¹ Manje Sara, mukazi wa AAAAAbrahamu, sana mu barile mwana eye, koma anali na wacito mukazi. Munthu waku Ejipito, wamene zina yake Aga. ² Ndipo Sara ana kamba na Abulahamu. ' Ona, Yehova anigwila ene kusakhala na bana. Enda uka gone na wacito. Ciga nkale kuti nizankhala na bana mwa eye." Abulahamu anavela ku mahu ya Sara, ³ pamene Abrahamu anankhala zake 10 mukanani pemozi na Sara, mukazi wa Abulamu, ana pasa aga, wacito wake waku Ejipito, mwa muna wake ku nkhalu mu kazi wake. ⁴ Sopano anli chibwezi na Aga, ndipo anankhala namimba. Pamene ana ona kuti ana kuti ankhala namimba. Ana nkhalu na chifukwa na omulemba wachito wake. ⁵ Ndipo Sara anakamba na Abrahamu, " Uku kulakwa kwanga chifukwa cha ewe. Ni nakupasa wachito wanga mukazi kuti ukale naye, pame anaona kuti ankhala namimba omulemba chito wake. Sinina muko dwelese mu maso yake. Leka Yehova a weluze pakati paine na ewe. ⁶ Koma Abulamu anakamba kuli Sara, " Ona pano, wachito wako muzimai ali mu manja yako. Chita na eve chimane uganiza uza ku wamiza. " Sopano Sara ana chita mwankhaza na eve, ndipo anataba kuchoka kwa eve. ⁷ Mu ngelo wa Yehova ana mupeza mu bali ya manzi muchipululu, mu bali ya mumanzi pajila Suri ⁸ Ana kamba, " Aga, wachito wa Sara, uchikelekuti ndipo uyenda kuti? " Ndipo ana yanka kuti, " Nili kutaba kuli unilemba chito wanga." ⁹ Mu ngelo wa Yehova ana kamba nae. " Bwelela kuli okulemba chito wako. Zipeleke na kuzi chepesa ku ulomulilo wake." ¹⁰ Ndipo mu ngelo wa Yehova ana kamba nae, " ni zaku chulukisa kwabili obabadwa kwaiwe. Kutu ba ka khale bubili ochuka osabelengeka." ¹¹ Mu ngelo wa Yehova anakambaso naye. " Onani, wankala na mimba uzakara na mwana mwamuna. Ndipo uza mu etana Zina Ishmaeli. Chifukwa Yehova a vera kuvutisika kwako. ¹² Aza nkhalu munthu. Ngati bulu wamu sanga, azakhala osa velana na munthu aliyese, ndipo aza siyana naba bale wake." ¹³ Ndipo anapase zina iyi kuli Yehova wamene kamba naeye, "Ndiwe Mulungu wamene uniona ine," ndaba ana kamba, " Kodi ne pitiliza ku ona, ngankhale pa buyo poni ona ene? " ¹⁴ Kwaichoo chi ceme china itanidwa Beaya Roi, Onani, chili pakhati Kadesh ndi Beredi. ¹⁵ Aga ana bara mwana mwamuna kwa Abram, ndi Abram anamupa zina mwana wake mwamuna wamene Aga anamu barila, Ishmaeli. ¹⁶ Abrahamu anali ndi zaka Eite sikisi pamene Aga ana bara Ishmaeli kwa Abram.

Chapter 17

¹ Pamene Abram u anali ndi zaka naite naine, Yehohova anaonekela kuli Abram ndipo anakamba, "Ndine Mulungu wamphavu zonse. Yenda pamanso panga, ndipo nshala ulibe chifukwa." ² Ndipo ndizasimikiza mapangano yanga ndi ine, ndipo muzapaka nakupitilila." ³ Abram anagwada moika wake pansi ndipo mulungu anakamba naye, nati, ⁴ "Kwaine, ona, chipangano changa chili naiwe. Unkhala tate wamaiko ambili." ⁵ Zina yako sizankhala Abram, koma izakahala Abrahamu ndipo nakusankha unkhala tate wamaiko yambili. ⁶ Ndizakubalisa iwe zaona, ndipo nizapanga mitundu yambili kuchoka mwaiwe, ndipo mafumu azabadwa kuchokela kuli iwe. ⁷ Nizapanga chipangano pakati pa iwe na ine na obadiwe pambuyo iwe mumibado yao yonse kwa chipangano chamuyayaya, kukhala mulungu wako na obadwa kwa iwe pa mbuyo pako. ⁸ Nizakupasa iwe, na obadwa kwa iwe pa mbuyo pako, malo amene mukhalamo, malo yonse yamu canaan, malo yamene muzakhala nayo kwamuyayaya ndipo nizankhala mulungu wabo." ⁹ Ndipo Mulungu anati kuli Abrahamu, "Iwe, ufunika kusunga chipangano, iwe na obadwa kwaiwe pa mbuyo pako mumibado yao yonse." ¹⁰ Ichi ni chipangano changa, chamene iwe ufunika kusunga, pali ine na iwe na obadwa kwa iwe pa mbuyo pako: Amina bonse bafunika kudulidwa. ¹¹ Bafunika kudulidwa khanda yakusogolo, na ichi chizankala chitsazo chachipangano changa pali ine na iwe. ¹² Bana bonse bamuna bali namatsiku eyiti afunika kudulidwa, mumibado zabantu bako bonse. Kuikilapo na onse obadwa munyumba mwako na iwo amene aguliwa na ndulama kuli alendo amene si obadwa kwa iwe pa mbuyo pako. ¹³ Mwamuna amene abadwa munyumba mwako na wamene waguliwa na ndalama afunika kudulidwa. Mwaicho chipangano changa chizankhala mu nkhandu yano mu chipangano chosavila. ¹⁴ Mwamuna aliyense wamene sanadulidwe na mu dulidwe wakanda yakusogolo afunika kuchotsedwa pakati pa bantu bake. Apwanya chipangano chonga." ¹⁵ Mulungu anakamba kuli Abrahamu kuti, "Mukazi wako Sara, osamuitana futi Sarai. Koma Sarah. ¹⁶ Nizamudalitsa, ndipo nizakupasa mwana mwamuna muli yeve. Nizamudalitsa, ndipo azankhala mai wamaiko ambiri. Mamfumu abantu azachokela kwa yeve." ¹⁷ Abrahamu anagwada nakuika mutu wake pansi, nakuseka ndipo anakamba mumtima wake, "Kodi mwana angabadwe kuli mwamuna alinazaka handiedi? Nizontheka bwanji Sarah, alinazaka naite, kubala mwana mwamuna?" ¹⁸ Abrahamu anakamba kuli Mulungu kuti, "Ishmaheli azankhalila pamaso panu!" ¹⁹ Mulungu anati, "Iyayi, koma mukazi wako Sarah azakubalira mwana wamwamuna, ndipo uzaka mupasa zina ya Isaki. Nizakhazikisa chipangano changa ndi iye chifukwa chipangano ndi chamuyayaya na obadwa pa mduyo pake." ²⁰ Pali Ishmayeli, nakubvela. Ona, namu dalitsa iye ndipo nizamupanga kuchuluka kwambili. Azakhala tate wabana twove achimu amfumu ndipo azakhala dziko yaikulu. ²¹ Koma chipangano changa niza khazikisa ndi Isaki, wamene Sarah azakubalira iwe pa nthawi ino chaka chitubwera." ²² Pamene anasiliza kukamba nayo, Mulungu anachokapo pali Abrahamu. ²³ Abrahamu anatenga Ishmayeli mwan wake mwamuna, na bamene bonse banabadwila mumfumba mwake, na bamene bonse banali munyumba mwa Abrahamu, ana dulidwa khanda yao ya kutsogolo pa tsiku yamene ija, monga mwamane mulungu anakambila naye. ²⁴ Abrahamu anali ndi naite naine zaka zaku badwa pamene anadulidwa khada yaka yakutsogolo. ²⁵ Ishmayeli mwana wake anali ndi zaka satini pamene anadulidwa khanda yake yakutsogolo. ²⁶ Patsiku imene ija Abrahamu na Ishmayeli mwana wake mwamuna anadulidwa. ²⁷ Amuna onse amumumba mwake anadulidwa naye, pamozi nabonse bana badwila munyumba na bonse bamene banagulidwa na ndalama tuchokele ku maiko yene.

Chapter 18

¹ Yehova anaonekela kwa Abraham pa mtengo wa Mamre, pamene anankhala pa ciseko pa kazuba ka siku. ² Anayanga kumwamba ndipo, onani anaona bamuna batatu baimilila pasogolo pake. Pamene anabaona, anathamanga kukumana noa kucoka pongenela pa nyumba na kugwanda kuika mu wake pansi. ³ Anati, "Ambuye banga, ngati napeza mwai mumenso mwanu, napapata musapitilire wanchito wanu." ⁴ Lekani manzi yang'ono yabwekesewe, sambani kumendo, pumulani pansi pa mtengo. ⁵ Lekani nibwelese cakudya cing'ono, kuti muzipumulise imwe mweka. Kucoka apo mungayende, pakuti mwabwelela kwa wanchito wanu. " Bananyankha." Cita monga mwamene wakambila. ⁶ Ndipo Abrahamu Anayenda kuli Sara mofulumila, naku muuza kuti, "Endesa, tenga mapimo yatatu ya fulaulo, panga fulawa, upange buledi." ⁷ Pamene apo Abrahamu anathamanga kuyenda ku ng'ombe, nakutenga kang'ombe kamwana kamene kanali kabwino, nakumupasa wanchito, wamene anaenda kukakonzwa chakudya. ⁸ Eve anatenga mafuta yonunkira na mukaka, na kamwana kang'ombe kamene kanali kanakonzewa, nakuyika chakudya pasogolo pabo, ndipo anayimirira pafupi nawo pansi pa mtengo pomene beve banali kudya. ⁹ Ana mufunsa kuti, "Nanga Sara mukaziwako alikuti?" Anayanka kuti, "Ali muja, muhema." ¹⁰ Ndipo anakamba kuti, Nizabwera kuli iwe nthawi yamasika, ndipo onani, Sara mukazi wako azakankala na mwana mwamuna. Sara apo anali kumvelera pakomo ya hema yamene inali kumbuyo kwake. ¹¹ Manje Abulahamu na Sara banali banakalamba ndipo banali na zaka zobadwa zambili, na Sara anali atapitirira msinkhu wobala bana. ¹² Ndipo Sara anaseka m'mtima mwake, nakukamba mumtima mwake kuti, Pamene nankala nkalamba ine nika pezemo kusangalala?" ¹³ Yehova anakamba kuli Abrahamu kuti, Nanga nichifukwa chani Sara aseka nakukamba kuti, Nanga nizankala na mwana pamene nakalamba? ¹⁴ Nanga kuli chamene akangiwa Yehova? Ntawi ngati yamene ino chaka chamene chibwela Sara azankala na mwana mwamuna." ¹⁵ Koma Sara anakana, kukamba kuti, Sininasekeko ine, chifukwa anayopa. Eve anamuyanka kuti, "Iyi, iwe wenze waseka." ¹⁶ Pamene apo bamuna baja bananyamuka kuti bayende moyang'ana Sodomu. Abrahamu adaenda nabo kukabapelekeza munjira. ¹⁷ Koma Yehova anakamba kuti, "Kansi nimubise Abrahamu chamene nifuna kuchita," po ona kuti Abrahamu azankala mtundu ukulu wamphamvu, ndipo mitundu yonse zapa ziko yapansi zizadaliska muli eve? ¹⁸ Pakuti ninamusanka kuti alangize bana bake, na banja yake ya kumbuyo kwake, kuti basunge njila ya Yehova, kuchita chilungamo na chiweruzo, kuti Yehova afikilize kwa Abrahamu vamene anakamba na eve. ¹⁹ Pamene apo Yehova anakamba kuti, "Chifukwa chakuti kulira kwa Sodomu na Gomora nikukulu, ndipo chifukwa chimo yawo niyayi kulu maningi, ²⁰ nizaselukila kwamene kuja, kuti nikazionele kulila koshushana nayeve kwamene kwabwela kuli ine, ngati nimwamene mwachitikila. Ngati simwamene, nizaziba." ²¹ Pamene apo bamuna baja banapindamuka kucokela kwamene kuja, nakuyenda ku Sodomu, koma ²² Abulahamu anasala ali imilile pamanso pa Yehova. Abrahamu ana fendela pafupi nakukamba kuti, "Manje muzawononga bolungama pamodzi na bantu boipa?" ²³ Kapena balimo bolungama makumi yasanu mukati mwa mzinda wamene uyu. Nanga muzai ononga yonse, mosayasiya malo aya chifukwa cha bolungama bali makumi yasanu bamene bali mwamene muja?" ²⁴ Chinkale kotalitali naimwe kuti muchite chamene ichi, kupaya bolungama pamozi na boipa, kuti bolungama nabeve bachiwe munjila imozi. Chinkale kotalitali na imwe! Nanga muweruzi wa ziko yonse yapansi sazachita cholungama?" ²⁵ Yehova anakamba kuti, "Nikapezamo m'Sodomu bolungama makumi yasanu mukati mwa munzi, nizayasunga malo aya chifukwa chao." ²⁶ Abrahamu anayankha nakukamba kuti, "Onani, nachitenga pali ine kukamba naba Ambuye banga, ngakale kuti ndine doti na milota." ²⁷ Manje ngati kuzakala chabe bolungama bosakwanila makumi yasanu? Nanga muzawononga muzinda wonse chifukwa cha kupelebeli bantu basanu?" Anamuyanka kukamba kuti, "Sininga yese kuwu wononga nikapezako makumi yanayi na yasanu." ²⁸ Ndipo anakamba nafuti kuli eve kuti, Nanga bakapezekamo chabe makumi yanayi mwamene muja? Eve anamuyanka kuti, "Sinizachita chifukwa cha makumi yanayi yamene ayo." ²⁹ Ndipo anakamba kuti, Musakalipe, Ambuye, kuti ine nikambe. Nanga mukapezeka chabe kuti muli bali makumi yatatu mwamene muja." Eve anamuyanka kuti, "Sinizachichita, nikapeza makumi yatatu mwamene muja." ³⁰ Ndipo anakamba kuti, Onani, nakamba ba ba Mbuye banga! Manje kapena mwapezeka makumi yabiri mwamene muja. Eve anayanka kuti, "Sinizawononga chifukwa cha makumi yabili ayo." ³¹ Anakamba kuti, "Nipempa kuti, musakalipe, Ambuye, ndipo ndipo nizakamba kosiliza. Mwina kapena ni kumi chabe bamene bazapezekamo mwamene muja." Pamene apo anamba kuti, "Sinizawononga chifukwa cha kumi." ³² Ndipo Yehova anaenda njila yake pamene anasiliza kukamba na Abrahamu, na Abrahamu anabwerera kuyenda kunyumba kwake.

Chapter 19

¹ Ba ngelo banabwela ku Sodom kumazulo, pamene Loti enzenkale pongenela mu muzinda wa Sodom. Pamene Loti anabawona, ananya mukka kuyenda kubatumanya, anangwada no paka mutu wake pansi. ² Anakamba kuti, "Napapata bakulu banchito yanga, niku pempani kuti mubwele kuny' umba kwa wa chitowanu, munkale usiku, musambe naku meendo. Munganya muke kuseeni noyenda njila yanu." Bana yaanta, "Iyayi, tizagona pano pangila." ³ Anapapata cho koselela, banayenda na yeve nongena munyumba. Anakoza zokudya nopanga mukate ulibbe vopakisa, ndipo banadya. ⁴ pe bakalibe kogona, bamuna ba mumuzida, bamuna bamu Sodomu, bana zinguluka nyumba bana nabakulu bamuna boonse bamumizinda yonse. ⁵ Bana yitana Loti, banati kuli yeve, "balikuti bamuna bamene babwela kuli iwe usiku uno? balete kuli ise, tibazibe." ⁶ Ndipo Loti ananyenda panja pachiseko no vala chiseko kumbuyo kwake. ⁷ Akamba, "Namimpempani abbale banga, musachite zo chimwa." ⁸ wayonani, nilina bana bakazi babili bekakalibe kuziba mwamuna. nivomeleseni, niku papatani, kuti nibalete kuli imwe, ndipo muzachita zo kondwelesa aba, chifukwa bamu chinvili chamutenge wanga." ⁹ Banati, "bwelela mumbuyo! "Bana kamba nafuti, "uyu anabwela kunkala wachilendo, manje afina kunkala woweluza wata! Manje tizamuchita zoyipa kuchila beve." Banalimbana naye mwa muna, banalimbana na Loti, ndipo bana bwela pafupi kufuna kupwanya chiseko. ¹⁰ Ndipo bamuna banachosa kwanja no donsele Loti munyumba kuli beeve no vala chiseko. ¹¹ Balendo ba Loti bna vela menso ya bamuna benze panja pa chiseko cha myumba, bana na ba kulu, ndipo banalema pe benzo josa kusakila chiseko. ¹² Bamuna banakamba kuli Loti. "uliko nawuliwonse pano? Mupongozi mwamuna, mwana mwamuna, mukazi na uliwonse wako mumuzinda, bachose pano." ¹³ Tifuna kuwononga malo ano, chifukwa kulila kwawo kwavenka mamingi kuli yehova ndipo atituma kuti tiwononge malo ano." ¹⁴ Loti anayenda kukamba na azipongizi bake bamuna, bamuna bana lonjeza kukwala bana bake, anati, musanga, chokani pamalo aya, chifukwa Yehova afuna kuwononga muzinda. "Kubapongozi bake bamuna chinawoneka monga a seka. ¹⁵ Pamene kunacha, angelo anawuza Loti, kuti, "yambani kuyenda, tenga mukazi wako na bana bako bakazi bali pano, musanyekele pamozi na chilango chamuzinda." ¹⁶ Anawayawaya. Ndipo bamuna bangwila kwanya kwake, kwanga kwamukazi wake, namanja yabana bake bakazi kuchoka mumuzinda. ¹⁷ Pebanabachoza panja, mwamuna umonzi anati, "Tamangilani umoyo wani! musayangene kumbuyo, usankale mumalo yalibe kantu kalikonse. Tamangila kulupili kuti musa nyeke." ¹⁸ Loti anati kuli Beeve, "iyaye, napapata, bakulu banchito yanga! ¹⁹ Wanchito wanu apeza chisomo pamenso yanu, anso mwanilangisa chifundo chopitilila mukupulumusa umoyo wanga. Ndipo siningtamangile kulupili, chifukwa chiwonongeko chachikulu chinganipeze, ndipo nizafa. ²⁰ Wona, uja muzinda alipafupi maningi kutabilako, anso nikang'ono napapata, lekani niyenda (sikangono?), Ndipo umoyo wanga uzapuluma. ²¹ Anamuwuzu iye, "Chabwino, Nivomekeza pempo iyo, siniza wononga muzinda ye wakamba. ²² Yendesa! tanamanga kja, sinizachita chilichose paka ufikeko." Ndipo uyu muzinda unali zowa. ²³ Pamene zuba inekwele pa ziko Loti anali anafika ku Zowa. ²⁴ Yehova analokesa nvula ya Saufa mu mulilo kuchokela kumwamba mu sodom na Gomora. ²⁵ Ana wononga mizinda zija, an malo yalibe kantu kalikoonse, nazonse zamoyo zinanili mumuzinda, nazonse zomela pansi. ²⁶ Ndipo mukazi wa Loti, anali kumbuyo kwake, anayangana kumbuyo, ana sanduka cuulu cha saulti. ²⁷ Abrahamu ananyamuka kuseni, no yenda pa malo pamene enze anayimilila ana Yehova. ²⁸ Anayanga pansi ku Sodoma na Gomora nowona, chusi chinyamuka kuchioka pansi monga chusi chamu fanasi. ²⁹ Pomwe Mulungu ana wonnga muzinda wa maloyalibe chilichonse, Abrahamu anabwela mumaganizo ya Mulungu. Anatuma Loti kuchoka pakati pa chiwonengeko pamene anaeononga muzinda wamene Loti analikunkalamo. ³⁰ Koma Loti anachoka mu Zowa kuyenda kunkala kupili nabana bake babili bakazi, chifukwa anali na manta kunkala mu Zowa. Anankhala mu cimubo ca mulipili. Eve na bana bake bakazi. ³¹ Mwana woyamba anawuza mufana wake, "batate bakakota, kulibe bamuna konse kulibe mwamuna azagona naise monga mweba machitila pa ziko la pansi. ³² Bwele, tiye timwese batate moba, ndipo tizagona nabo, kuti tusunge mbewu ya batate batu." ³³ Uja usiku banapasa batate bawo moba. Ndiponso woyambila anayenda nongona nabatate bake; batate bake sibanazibe pe anagona, na pe anawuka. ³⁴ Sikuyokonkapo woyambila anawuka mung'ono, "nvela, nonangona nabatate usiku wapita, Tiye tibamwese moba lelo usiku nafuti, ndipo uzayenda kugona nabo, kuti tisunge mbwe yabatate batu." ³⁵ Uja usiku nawo banapasa batate bawo moba, ndipo mung'ono anayenda kugona nabatate bawo. Batate bake sibanazibe pe anagona na pe anawuka. ³⁶ Bana bonse babili ba Loti banankala na mimba yabatate bawo. ³⁷ Woyambbila anabala mwamuna, ndipo anamupasa zina Mohabu. Anankala kolo wana Mobaiti balelo. ³⁸ Ndipo mupana wake, anabala mwana mwamuna, no mupasa zina la Ben-ammi-nchipo anankala kolo wa mantu ba Ammoni ba lelo.

Chapter 20

¹ Abrahamu anacokako kuja kupita ku malo ya Nagev, ndipo anankhala pakati padesi na suri. Enze mulendo wonkhala mu Gerari. ² Abrahamu anakamba pali Sara mkazi wake, "Uyu ninabadwa naye." Abimeleki mfumu ya Gerari anaitana Sara na kumtenga. ³ Koma Mulungu anabwela kwa Abimeleki mu maloto usiku, na kuti kwa eve, "Ona, ndiwe munthu wokufa cifukwa ca mkazi wamene watenga, pakuti ni mkazi wa munthu." ⁴ Manje Abimeleki sanabwele pafupi na eve ndipo anakamba kuti, "Ambuye, munga paye ziko yalungama?" ⁵ Sanakambe eve eka kwa ine, 'ninabadwa naye, 'Nacita ici mwa ulemu wa mtima wangu na kupanda cifukwa kwa manja banga." ⁶ Ndipo Mulungu anakamba kuti kwa eve m'maloto, "Ee, niziba naine kuti mu ulemu wa mtima wako wacita ici, ndipo naine ninakulesa kunicimwila. Mwaici sininakuvomeleze iwe kuti umugwire." ⁷ Mwaici, bweza makazi wa munthu, pakuti ni mneneri. Azakupemphelera, ndipo uzankhala moyo. Koma ngati sumubwezela, ziba kuti iwe na ose amene uli nao zoonza muzafa." ⁸ Abimeleki ananyamuka kuseni seni na kuziitanila banhito. Anabauza ivi vinthu vonse kwa beve, na banthu banacit mantha. ⁹ Ndipo Abimeleki anaitana Abrahamu na kukamba kuti, "Nican camene wacita kwa ise? Nakucimwila bwanji, kuti wanibwelesela ine ufumu wanga cimo ikulu? Wanicitila camene siwenzofunika kucita." ¹⁰ Abimeleki anakamba kuti kwa Abrahamu, "Unaona cani kuti ucite ici cinthu?" ¹¹ Abrahamu anakamba kuti, "Cifukwa ninaganiza, 'zoonza mulibe kuyopa mulungu mu malo muno ndipo bazanipaya cifukwa ca mkazi wanga.' ¹² Pakuti, zoonza ninabadwa naye, ni mwana mkazi wa batate banga, koma osati mwana mkazi wa amai banga; ndipo anankhala mkazi wanga." ¹³ Pamene Mulungu ananilengesa kucoka pa nyumba ya batate banga na kuyenda kucoka ku malo aba kupita pa malo pena. Ninakamba kuti kwa eve, 'ufanika unilangize kukhulupilika kwako monga mkazi wanga: Pamalo paliponse pamene tizayenda, ukambe za ine, "Ninabadwa naye." ¹⁴ Ndipo Abimeleki anatenga mbelele na ng'ombe, na akapolo bamuna na bakazi, na kubapeleka kwa Abrahamu. Ndipo anambwezela Sara, mkazi wa Abrahamu, kwa eve. ¹⁵ Abimeleki anakamba kuti, "Ona, malo bangaali m'manja mwako. Nkhala paliponse pamene pazakukondwelesa." ¹⁶ Kwa Sara anakamba kuti, "Ona, napasa wobadwa naye wako ma sauzande ya silive. Ici nikuvinikila zolakwa pali iwe mu menso mwa onse bali na iwe, na pamenso pa aliyense, wapangiwa wonkhalilatu wolungama." ¹⁷ Ndipo Abrahamu anapemphela kwa Mulungu, ndipo Mulungu anapolesa Abimeleki, mkazi wake, na bakapolo bake bakazi kuti bakwanise kunkhale na bana. ¹⁸ Pakuti Yehova analengesa onse bakazi ba mnyumba mwa Abimeleki bankhaliletu osabala, cifukwa ca Sara, mkazi wa Abrahamu.

Chapter 21

¹ Yahova anaikako nzelu kuli Sara monga mwamene ana kambila, na Yahova anachitila Sara vamene ana kamba.

² Sara ana nkhalana na mimba nakubala mwana mwamuna wa Abrahamu mu ukhalamba wake pa nthuwi yamene Mulungu ana kamba. ³ Abrahamu anamu pasa zina mwana wamene kuli eve, wamene Sara anamu balila, Isaki. ⁴ Abrahamu anamu duka mwana wake Isaki pamene ana kwanisa masiku eiti, monga mwamene Mulungu ana lamulila kuli eve. ⁵ Abrahamu anali ana zaka handiladi pamene mwana wake Isaki anabandwa. ⁶ Sara anati, "Mulungu ani lengesa ku seka; bonse banza nvela baza seka naine." Ni ndani ana ganizila kuti. ⁷ Ndiposo Sara anati, "Ni ndani ana ganizila kuti Sara anga nkale na bana koma namu balila mwana mwamuna mubu nkalamba wake. ⁸ Mwana ana kula nakuleka ku nyonkha ndipo Abrahamu ana panda chikondwelelo chachikulu pamene ana siya ku nyoka Isaki. ⁹ Sara ana ona mwana wa Haga waku Egipito, wamene ana balila Abrahamu amuseka. ¹⁰ Tsopano anati kuli Abrahamu, "Mu choseni pano kapolo na mwana wake, chifukwa mwana wa kapolo saza nkala oloba pamodzi na mwana wanga Isaki." ¹¹ Ichi chinamu nkhalila chomu vitisa abrahamu chifukwa cha mwana wake. ¹² Ndipo Mulungu anati kuli Abrahamu, "Osa nkala ovutisiwa chifukwa cha mwana, na kapolo wako. Nvele mau yake yonse yamene akamba pali iyi nkani, chigukwa ni muli Isaki mwamene bonse bodwa bakupaza pasiwa zina.

¹³ Ndipo niza pangaso mwana wa kapolo mukazi ziko, chifukwa nobo badwa wako. ¹⁴ Ndipo Abrahamu anacita kuseni, naku tenga mukate na chikumba cho tengelamo manzi, naku pasa Haga no ika mwana pamusana pake. Ana yenda ku chipululu ku Bereseba. ¹⁵ Pamene manzi yanasila muchi kumba cho tengamo manzi, anasiya mwana munsu mwa mtengo. ¹⁶ Ana yenda, ankala patali na mwana, mutunda wa Muvi, anazi kambisa eka, nisaoneko kufa kwa mwana wanga, "Ndipo ana nkhalapo oneka naye, ana bwela ayamba kulilamo kuwa. ¹⁷ Mulungu anamvela kulila kwa mwana, ndipo mungeli wa Mulungu anaitana kuli Haga ku chokela ku mwamba, naku kamba kuli eve, "Ni chani chaku vuta, Haga? Osa yopa chifukwa Mulungu anamvela kulila kwa mwana kwamene alili. ¹⁸ Nyamuka imika mwana nakumulibisa: chifukwa Nizampanga eve kunkhala ziko ikulu. ¹⁹ Ndipo Mulungu anamu segula menso, nakuona chisime cha manzi. Ana yenda nakuika manzi muchi tumba cha manzi, no pasa mwana kumwa. ²⁰ Ndipo Mulungu anali mwana uja, ndipo ana kula. Ana nkala mu chipululu Nunkhala wopaya nyama. ²¹ Ana nkala mu chipululu cha Parana, ndipo amai bako anamu tengela mukazi waku malo ya Egipito. ²² Ina fika ntawi pamene Abimeleki na Fikolakulu ankonda ana kamba kuli Abrahamu kuti, "Mulungu ali na iwe mu vonse vamene uchita. ²³ Tsopano vomele na ine pa Mulungu kuti suza chita boza na ine, olo bana banga nangu bonse bo badwa kuli ine. Ni langize malo yemene unali ku nkalamo monga wachilendo mubu bwino chimozi mozi. ²⁴ Abrahamu anati, "Na vomela." ²⁵ Abrahamu ana dandaula pali chisime chamene anamupoka kuli anchito ba Abimeleki. ²⁶ Abimeleki anati, "Siniziba wamene ana chita ivo. Koma futi sunai uzepo; panka apa manje." ²⁷ Ndipo Abrahamu ana tenga mbelele na ng'ombe naku pasa Abimeleki, na amuna abili naku panga chi pangano. ²⁸ Tsopano Abrahamu ana tenga bana ba mbelele seveni zikazi naku zi ika [a zeka. ²⁹ Abimeleki anati kuli Abrahamu, "Tantauzo ya izi nyama zamene wa ika pa zeka ni chiyani? ³⁰ Ana yankha tenga mu manja mwanga zizani nkhalila umboni, kuli nina kumba chisime." ³¹ Ndipo malo aya anaya ita beresheba, chifukwa bonse babili bana panga lonjezo. ³² Ana panga ma panyano pa Beresheba, na Abimeleki na Fikol, mukulu wa nkonda, ana bwelela ku malo ya filisiti. ³³ Abrahamu ana shanga chi mtengo cha tamariski ku Beresheba. Napamene apo ana pempeza Yahova, wamuyayaya Mulungu. ³⁴ Abrahamu ana nkala wachi lendo mu malo ya Filisiti masiku yambili.

Chapter 22

¹ Pamene ivi vinapita Mulungu anayesa Abrahamu. Anamu uza kuti, "Abrahamu!" Abrahamu anayanka kuti, "Ine nili pano." ² Mulungu anakamba kuti, "Mutenge mwana wako, mwana mwamuna wako eka, wamene ukonda, Isaki, uyende ku malo ya Molaya. Umupase ankale nsembe yoshoka pa pili imozi yakuja, yamene nizaku uza." ³ Mwa ichi Abrahamu anaima kuseni-seni, anakwela bulu yake, anatenga banyamata babili bang'ono pamozi na eve, na Isaki mwana wake. Anatyola mitengo zopelekelapo nsembe, nanyamuka ulendo kuyenda kumalo kwamene Mulungu anamu uza. ⁴ Pa siku yachitatu Abrahamu anaimya menso nakuyaona malo pataliko. ⁵ Abrahamu anauza banyamata bake kuti, "Lindilani pamene pano na bulu, ine na munyamata tiyenda apo. Tizapembeza naku bwela futi kuli imwe." ⁶ Abrahamu anakonza nkuni za nsembe naku ikapo mwana wake Isaki. Ananyamula kumanja mulilo na lupanga; ndipo bana enda pamozi. ⁷ Isaki anauza Abrahamu tate wake kuti, "Batate banga," ndipo banamuyanka kuti, "Ine pano, mwana wanga." Anakamba kuti, "Onani, uyu apa mulilo na nkuni, manje nanga kamwana ka nkosa kopeleka nsembe kali kuti?" ⁸ Abrahamu anayanka kuti, "Mulungu azapeleka eka mwana wankosa wa nsembe yo ocha, mwana wanga." Mwamene umo banaenda, bonse babili pamozi. ⁹ Pamene banafika pamalo yamene Mulungu anamuwuzapo eve, Abrahamu anamanga guwa yansembe pamene apo na kuyikapo nkuni zija. Pamene apo anamangilila Isaki mwana wake, nakumugoneka paguwa yansembe, pamwamba pa nkuni. ¹⁰ Abrahamu anatambasula kwanja kwake nakutenga mupeni kuti apaye mwana wake. ¹¹ Ndipo mungelo wa Yehova anamuitana eve kuchokera kumwamba kukamba kuti, "Abrahamu, Abrahamu!" ndipo anati, "Ine pano." ¹² Eve anakamba kuti, "Usaike kwanja yako pali munyamata uyo, kapena kumuchita chilichonse choipa, chifukwa manje naziba kuti iwe uyopa Mulungu, popeza kuti sunanikanile ine mwana wako, mwamuna wobadwamo eka." ¹³ Abulahamu anaimya menso yake ndipo, onani, kumbuyo kwake kunali nkosa yamphongo yamene inagwiliwa na nsengo zake. Abulahamu anaenda kukaitenga nkhosa yamene ija na kuipeleka monga nsembe yopsereza mumalo mwa mwana wake. ¹⁴ Ndipo Abrahamu anaitana malo yamene yaja kuti ni "Yehova azapeleka", kufikila na lelo, "Pamwamba pa lupili ya Yehova vizapasiwa." ¹⁵ Mungelo wa Yehova anaitananso Abrahamu kachibili kuchokera kumwamba, ¹⁶ naku kamba kuti- "Yehova akamba kuti, Ine nalapa pa ine kuti chifukwa wachita chintu chamene ichi, kosanikanila mwana wako mwamuna umozi eka, ¹⁷ nizakudalisa Nizachulukisa mbewu zako monga nyenyezi za kumwamba, na monga muchenga wa mumbali mwa nyanja; ndipo mbewu zako zizatenga chipata cha adani awo. ¹⁸ Kupitila mwa mbewu yako, mitundu zonse zapa ziko yapansi zizadalisika, chifukwa wamvera mawu yanga." ¹⁹ Ndipo Abrahamu anabwelela kuli banyamata bake, ndipo anachoka nakuyenda bonse pamozi ku Biyasheba, ndipo eve anankala ku Biyasheba. ²⁰ Chinachitika kuti pamene ivi vinapita banamuza Abrahamu kuti, Milika nayeve anabala bana kuli mubale wako Naholi. ²¹ Aba banali mwana wake woyamba Uzi, mubale wake Buzi, Kemuweli anabala Alamu, ²² Kesedi, Hazo, Piludashi, Yidilafu na Betuele. ²³ Betuele anabala Rabeka. Aba ndiye bana basanu na batatu bamene Milka anamubalira Naholi mubale wa Abrahamu. ²⁴ Mukazi wake wamung'ono, dzina yake Reuma, anaba nafuti Teba, Gahamu, Tahasi na Maaka.

Chapter 23

¹ Sarai anankhala zaka 127. Izi ndiye zaka zawumoyo wa Sarai. ² Sarai anafela mu Kiriti Arba, ndiye kuti, Hebroni, muziko ya Kenani. Abrahamu ana dandaula na kulila Sara. ³ Pamene apo Abrahamu anayamuka na ku cokako kwa mukazi wake wokufa, na kunena ku bana ba A'Hetu, kuti, ⁴ "Ndine mulendo pakati panu. Nipasenikoni malo ya manda pakati pa imwe, kuti ni ike wanga okufa." ⁵ Wana wa Heti bana muyankha Abrahamu, kuti, ⁶ "Tiveleni ife, bwana wanga. Ndimwe mwana wa mfumu wa Mulungu pakati katu. Ikani wokufa wanu mumanda yathu ya bwino. Kulibe amene azakulesa manda yake, kuti uyikemo wa kufa wako." ⁷ Abrahamu ananyamuka naku gwanda kubantu amudziko, kuli bana A'Hetu. ⁸ Iye anakamba nabo, kuti ngati imwe mwavomela kuti n ike bokufa wanga, manje ninveleni na kunimpepelako kuli Efulon mwana wa Zohari, kuli ine. ⁹ Muni funsileko kuti aningulise kavu ya Machipela, yamene alinayo, yamene ili kumapeto yakumunda wake. Pa mutengo wake wonse, anigulise powonekela ngati malo yoyikapo ba kufa." ¹⁰ Isapano Efroni anali anankhala pakati pa bana ba Heti, ndipo Efroni Mhiti anayanka Abrahamu mu manso ya bana ba Heti, na bonse bamene bana bwela mu geti yamu zinda wake, kuti, ¹¹ iyayi, bwana wanga, niveleni ine, naku pasani munda, na kavu yamene ili mukati. Nakupasa iwe pa manso ya bana ba banga. Nakupasa iwe kuti uyike okufa wako." ¹² Pamene apo Abrahamu anagwanda pa manso pa bantu a mudziko. ¹³ Anakamba na Efron mukuvelela kwa bantu bamu dziko, kuti, koma ngati mufuna, napapata niveleni. Nizalipila zamunda. Tengani ndalama kuchokela kuli ine, ndipo niza ika wokufa wanga kuja." ¹⁴ Efron anayankha Abrahamu, kuti ¹⁵ "Chonde, bwana wanga, niveleni ine. Ka malo ka nthaka ko kwanila muyeso wafolo handredi ma shekeli ya siliva, ni cani ici camene cili pakati pali ine na iwe? Ika wakufa wako." ¹⁶ Abrahamu anavelela kuli Efulon ndipo Abrahamu ana pimila Efulo muyeso wa siliva wamene ana tomola pokamba milandu nabana bamuna ba Heti, Folo handiledi ma shekelo ya siliva, kulinga na kapimidwe ka bwino kama londa. ¹⁷ Munda wa Efulon, wamene unali mu Machifela, wamene unali pa fupi na mamre, uyo ndiye yonse yamene inali mu munda na konse muma lile, vina pasiwa ¹⁸ Bana vingulisa kuli Abrahamu pa manso ya bana bamuna ba Heti, pali bonse bamene benze bana bwela mu geti ya mu zinda wake. ¹⁹ Pasongolo pake, Abrahamu ana yika thupi ya Sara mukazi wake mu kavu ya mu munda wa machipela, wamene uli pafupi na Mamre, uyu ndiye Hebloni, muziko ya Kanani. ²⁰ Ndipo munda na kavu vinalimo vina pasiwa kwa Abrahamu kuti vinkhale katundu wake woyikilamo malilo, kucokela ku bana ba muna ba Heti.

Chapter 24

¹ Manje Abrahamu anali anakula maningi ndipo Yehova anamudalisa Abrahamu muvinthu vonse. ² Abrahamu anati kwa wanchito wake, wamene anali mukulu pa nyumba yake ndiponso wamene anali kulamulila zonse anali nazo, "faka kwanja kwako pansi pa chibelo changa. ³ Ndipo nizakulapisa iwe pa Yehova, Mulungu wakumwamba, ndi Mulungu wapansi, kuti usakamutengele mukazi mwana wanga mwamuna kuchokela kwa Akenaniwo, mwamene napanga nyumba yanga. ⁴ Koma uzayenda ku Ziko yanga, kuli ba bale banga nakumutengela mukazi mwana wanga Isaki. ⁵ Wanchito anakamba naye kuti, nanga ngati mukazi sazafuna kunikonkha kuziko lino? Nizakamutenga mwana wanu ku Ziko kwamene munachokela imwe? ⁶ Abrahamu anamuuzza kuti, "uone kuti usakamutenge mwana wanga kwamene uko. ⁷ Yehova Mulungu wakumwamba, wamene ananitenga ine kuchoka kunyumba ya batate banga na ku Ziko laba bale banga wamene anakamba na ine na kulumbila kwa ine kuti, ku mbeu zako nizakupasa iyi Ziko,"wamene azatuma mungelo kuyenda pasogolo pako kuti akusogolele kutenga mukazi wa mwana wanga kwamene uko. ⁸ Koma ngati mukazi sazafuna kukukonkha iwe, uzankhala omasuka pakulapila kwanga. koma siufunika kutenga mwana wanga kwamene uko. ⁹ Ndipo wanchito anaika kwanja kwake pansi pa chibelo cha Abrahamu bwana wake, ndipo analapila kwa iye pa chintu chamene icho. ¹⁰ Wanchito anatenga kuchokela kwa bwana wake ngamira zili teni ndipo anayambapo. Anatenganso mpaso zosiyana siyana kuchokela kuli ba bwana bake. Ananyamuka na kuyenda ku gawo la Aramu Naharaimu, ku muzinda wa Nahori. ¹¹ Anagwadisa ngamira kunja kwa muzinda kuchisime cha manzi. Iyi inali ntawi yakumazulo pamene bakazi banachoka kuyenda mukutapa manzi. ¹² Ndipo anati, "Yehova, mulungu wa ba bwana banga ba Abrahamu, nipaseni kupambana ine lelo ndi kukulupilika kwanu muchipangano ndi Bwana wanga Abrahamu. ¹³ Onani, Ine naimilila pa chisime cha manzi, ndipo nana bakazi ba mu muzinda babwela mu kutapa manzi. ¹⁴ Lekani chichitike motele, nikauza musikana, "napapata bweza pansi mugomo wako kuti nimweko manzi, ndipo azakamba kuti, Imwa, ndipo nizamwesanso na ngamira; wamene uyo ankhale mukazi osankila kapolo wanu Isaki. Pali ichi nizaziba kuti mwalangiza kukulupilika kwa chipangano kwa bwana wanga. ¹⁵ Chinachitika kuti pamene akalibe kusiliza kukamba, Onani, Rebeka anachoka ndi mugomo wake pa pewa. Rebeka anabadwa kwa Batuele mwana wa mwamuna wa Milika, mukazi wa Nahori, mubale wa Abrahamu. ¹⁶ Uyu mukazi anali wabwino ndiponso anali namwali. Sanazibepo mwamuna. Anaselukila ku chisime, ndipo anazulisa mugomo wake nakukwela pamwamba. ¹⁷ Ndipo wanchito anatamanga kuti akumane naye nakukamba kuti, napapata nipaseko yang'ono manzi mu mugomo wako. ¹⁸ Anati, Imwa, bwana wanga,"ndipo anayendesa nakubweza pansi mugomo wake mu manja mwake nakumupasa cha kumwa. ¹⁹ Pamene anasiliza kumupasa chakumwa, anati, "Nizatapa manzi ya ngamira zako, mpaka zimwe zonse." ²⁰ Ndipo anayendesa na kuchosa mu mugomo nakufaka muchomwelamo, nakutamangila kuchisime mukutapa manzi ya ngamira zonse." ²¹ Mwamuna anamulangana iye osakamba kanthu kuona kuti kapena Yehova anamuyendesa bwino mu ulendo wake kapena iai. ²² Pamene ngamira zinasiliza kumwa, mwamuna anachosa mpete yapampuno ya golide kulemela kwake sikelo lateka, na vibili va golide vibango vaku manja kwake volemela teni lateka. ²³ Ndipo anafunsa, "Ndiwe mwana wa bandani? Niuze napapata, kodi kuliko malo kuli ba tate bako kunyumba tigoneko usiku? ²⁴ Anayankha kuti, Ine ndine mwana wa Betuele mwana wa wamwamuna wa Milika, wamene anabala kwa Nahori." ²⁵ Anamuuzza futi nati, tili na wambili uzu na vakudya ndiponso na malo yogonamo usiku. ²⁶ Mwamuna anagwada na kuyamika Yehova. ²⁷ Anati, adalisike Yehova Mulungu wa bwana wanga Abrahamu, wamene sanakane ku kulupilika kwa chipangano ndi chifundo chake mwa bwana wanga. Koma monga ine, Yehova anisogolela munjila ya kunyumba ya ba bale ba bwana wanga. ²⁸ Ndipo mukazi wachichepele anatamanga nakuuza baku nyumba ya ba Mai bake vonse vintu. ²⁹ Manje Rebeka anali na mulongsi wake zina lake Labani. Labani anatamangila mwamuna wamene anali kunja kumuseu waku chisime. ³⁰ Pamene anaona mpete ya pampuno ndi vibango vakumanja kuli kalongosi wake, na pamene ananvela mau ya Rebeka mulongosi wake, ivi ndiye vamene mwamuna aniuza, anayenda kuli mwamuna, ndipo onani, anaimilila na ngamira pa chisime. ³¹ Ndipo Labani anati, "bwela, Iwe wodaliska wa Yehova. Ni chani uimilila panja? Nakonza nyumba na malo ya ngamira." ³² Ndipo mwamuna anabwela kunyumba nakumasula ngamira. Ngamira zinapasidwa mauzu na vakudya, na manzi yanapasidwa kuti asambe kumendo na mendo yaba muna bonse banali naye. ³³ Banamukonzela vakudya, kuti adye, koma anati, sinizadya nikalibe kukamba vamene nifuna kukamba. "Koma Labani anamuuzza kuti, "Kamba." ³⁴ Anamuuzza kuti, ndine wa nchito wa Abrahamu." ³⁵ Yehova anamudalisa bwana wanga kwambili ndiponso niolemela. Anamupasa iye nkosa na ng'ombe, siliva na golide, ba nchito bamuna na bakazi, ndi ngamira naba bulu. ³⁶ Sara, mukazi wa bwana wanga, anabala mwana mwamuna kwa bwana wanga pamene bwana wanga anakota, ndiponso anamupasa vonse vinali vake. ³⁷ Bwana wanga ananilumbilisa ine kuti, usamutengele mwana wanga mukazi waku Kanani, mu malo mwamene ine ninkhala. ³⁸ Koma, uyende ku banja

ya batate banga, nakuli ba bale banga, nakutenga mukazi wa mwana wanga.³⁹ Nizamuuza bwana wanga, "nanga ngati mukazi sazanikonkha."⁴⁰ Koma ananiuza kuti, "Yehova wamene niyenda naye, azatuma mungelo na iwe nakukudalisa munjila yako, kuti umutengele mwana wanga kuchokela kuli ba bale banga na kuli ba banja ba batate."⁴¹ Koma uzankhala omasuka ku chipangano changa ukabwela kuli ba bale banga iye kuli iwe. Ndipo uzankala omasuka ku chipangano changa.⁴² Ndipo nafika lelo ku chisime cha manzi, nakukamba, Yehova, Mulungu wa bwana wanga Abrahamu, napapata, ngati muzaniyendesa bwino munjila yanga-⁴³ Nilipo pano, naimilila pa chisime cha manzi—lekani mukazi azabwela kutapa manzi, mukazi wamene nizauza, napapata nipaseko manzi yang'ono mu mugomo wako kuti nimwe."⁴⁴ Mukazi azaniuza ine, "Imwa, ndiponso nizapasa manzi na ngamira zako."lekani ankhale mukazi inu, Yehova, mwamusankha wa mwana wa bwana wanga!⁴⁵ Nikalibe kusiliza kukamba mumutima mwanga, Onani, Rebeka anachoka ndi mugomo wake pa pewa yake, na kuselukila ku chisime na kutapa manzi. Ndipo ninamuuza, napapata nipaseko manzi yakumwa.⁴⁶ Mwamusanga anatula mugomo wake pachipewa nati, "Imwa, ndiponso nizapasa ngamira zako manzi. Ndipo ninamwa, ndipo anamwesanso na ngamira."⁴⁷ Ninamufunsa nati, ndiwe mwana wa bandani? anati, ndine mwana wa Betuele, mwana wa mwamuna wa Nahori, wamene Milika anabala kwa Iye. Ndipo ninafaka mpete pampuno yake na vibango kumanja yake.⁴⁸ Ndipo ninagwesa nkope yanga na kulambila Yehova, na kutokozza yehova, nakudalisa Yehova, Mulungu wa bwana wanga Abrahamu, wamene ananisogolela ine munjila, kuti nikamupezele mwana mukazi wake wa banja ya bwana wanga wa mwana wake mwamuna.⁴⁹ Sopano, ngati muli okonzeka kulangiza chikondi cha zoona na chikulupililo kwa bwana wanga, niuzeni. Ngati iai, niuzeni, kuti nipatukile ku kwanja kwaku manja kapena kukwanja ya manzele.⁵⁰ Ndipo Labani ndi Batuele anayankha kuti, Ichi chintu chachokela kwa Yehova: Sitingakambe kwa iwe choipa kapena chabwino.⁵¹ Onani, Rebeka ali pamenso pako, mutenge ndipo uyende, kuti ankhale mukazi wa mwana mwana wa bwana wako, mwamene Yehova akambila."⁵² Pamene wanchito wa Abrahamu ananva mau yawo, anagwesa nkope pansu pamenso ya Yehova.⁵³ Wanchito uyu anatulusa zabwino za siliva na zabwino za golide, na vovala nakumupasa Rebeka. anapasanso mpaso zabwino kwa mubale wake nakuli ba Mai bake.⁵⁴ Ndipo iye na bamuna anali nawo ba nadya na kumwa. Banankhala kuja usiku bonse, ndipo pamene banauka kuseni, anati, nitumeni kwa bwana wanga.⁵⁵ Mubale wake na ba Mai bake banati, lekani mukazi mun'gono ankhale naife masiku yang'ono masiku yali teni.⁵⁶ Koma anabauza kuti, "musanichingilize, chifukwa Yehova ananidalisa munjila yanga. Nitumeni kuti ningayende kuli bwana wanga."⁵⁷ Banati, "tizamuitana mukazi wamung'ono nakumufunsa."⁵⁸ Ndipo banamuitana Rebeka nakumufunsa, "uzayenda nauyu mwamuna?"Iye anayankha, "Nizayenda."⁵⁹ Ndipo banamutuma kalongosi wawo Rebeka, pamozi naba nchito bake bakazi, muulendo wake pamozi ndi wanchito wa Abrahamu na banthu bake.⁶⁰ Banamudalisa Rebeka nati, "mulongosi watu, leka unkhale make wa bana wanu sauzandi ndi teni sauzandi, ndipo leka bana bako batenge makomo ya bonse bamene babazonda."⁶¹ Ndipo Rebeka ananyamuka, iye naba nchito bake bakazi nomanga pa ngamira, nakumukonkha mwamuna. Wanchito uja anamutenga Rebeka nakuyenda naye.⁶² Isaki anali kunkhala ku Negev, ndipo anachokela ku Beer Lahai Roi.⁶³ Isaki anachoka kuyenda mukuganiza mu munda kumazuloNdipo analangana kusogolo nakuona, Onani, kunali ngamira zinali kubwela." Rebeka analangana, pamene anaona Isaki, anaseluka pa ngamira.⁶⁴ Anauza wanchito wake, "Nindani uja mwamuna wamene ayenda mumunda kubwela kuti akumane naife?"⁶⁵ Wanchito anati, "Ni bwana wanga."Ndipo iye anachosa chovinikila kumenso, nakuzivinikila.⁶⁶ Wanchito anamuuza Isaki vonse vamenene anachita.⁶⁷ Ndipo Isaki anamubwelesa iye kunyumba kwa Sara amai bake, nakumutenga Rebeka, nakunkhala mukazi wake, ndipo anamukonda. Ndipo Isaki anatontozedwa pambuyo pa infa ya ba Mai bake.

Chapter 25

¹ Abrahamu a natenga mkazi wina, zina yake enze Keturah. ² Ndipo anambalira iye Zimirani, Yokisani, Medeni, Midiyani, Isibaki ndi Suwa. ³ Ndipo Yokisani anakhala taet wa Sheba na Dedani, bana ba Dedani banali ba Assyriarl, ndi Letosu, ndi Leum. ⁴ Bana ba Midian bamuna benze Ephari, Epheri, Harlok, Abida, na Eldaah, bonse aba benze bana ba Keturah. ⁵ Abrahamu anapasa Isaki vinthu vake vonse. ⁶ Koma pene enze namoyo, anapasa mphaso bana bamuna ba bakazi bake bang'ono naku batuma kuziko la kumawa, kubacosa kuli Isaki, mwana wake. ⁷ Aya ndiye yannali masiku yazaka zimene Abrahamu anakhala namoyo, zake 175. ⁸ Abrahamu anapema kosiliza ana walila nazaka zabwino zokolamba, munthu nkote namoyo okwana, anatengewa kuli banthu bake. ⁹ Isaki na Ishumaele bana bake, bana muika mumphanga isa makipela mu munda wa Ephrori mwana wa zohari mu hitati, yamene iri pafupi na mamure. ¹⁰ Munda wamene Abrahamu enze anangula kuli bana ba Heti. Ndiye Abrahamu na mkazi wake Sara banai kiwa. ¹¹ Pambuyo paimfa ya Abrahamu, mulungu anadalisa mwana wake Isaki, ndipo Isaki enze kunkhala pafupi na Beeri Lahai Roi. ¹² Ndipo aba ndiye benze bana ba Ishumaele, mwana wa Abrahamu yamene Hagara mu Egipto, kapolo wa Sara, anabalira Abrahamu. ¹³ Aya ndiye ynze mazina ya bana ba bamuna ba Ishumaele kulingana namwamene banabadwira: Nabioti woyamba wa Ishumaeli, Kedar, Adbeel, Mibsam, ¹⁴ Mishma, Duma, na MAsa, ¹⁵ na Hadad, Tema, Jetur, Naphish, na Kedemah. ¹⁶ Aba ndiye benze bana ba Ishumaele, ndipo ndiye yenze mazina yao, kulingana na mizi yao na misasa zao; akalonga 12 kulingana na mitundu yao. ¹⁷ Izi ndiye zaka zamoyo wa Ishumaele, zaka 137, ndipo iye anamwalira, ndipo anatengawa kuli bathu bake. ¹⁸ Ndipo banakhala, kuyambira ku Havilah na kufika ku Ashhuri, yamene ili pafupi na Egipto, monga iyenda ku Assirila. bankhala boyambana bekha bekha. ¹⁹ Ivi ndiye venze vocitika va Isaki, mwana wa Abrahamu, Abahamu ana bala Isaki. ²⁰ Isaki enzeli na zaka 40 pamene kwatira mkazi wake Rabeka, mwana wa Betuero mu Aramearl wa ku Paddors Arars, Mlongo wake wa Labari mu Aramearl. ²¹ Isaki anapemphelera mkazi wake kwa Tehova cifukwa senze kubala, ndipo Yehova anayankha pemphero yake, ndipo mkazi wake Rabekah anakhala navumo. ²² Bana banavutana muvumo mwake, ndipo anakamba kuti, "Cifukwa ni chani ivi vicitika kuli ine?" Ndipo anayenda kufusa Yehova pali ivi. ²³ Yehova anakamba nayeve, "Maziko yabili yali mu vumo mwako, Mangulu yabili ya banthu ya zachoka muli iwe, gulu izakhala ya mphavu kucila inzake, ndipo mkulu azakhala kapolo wa mufana." ²⁴ Pamene nthawi yobala inakwana, Taonani, mwenze ba mpundu mu vumo. ²⁵ Mwana woyamba anacoka wofiila monse monga chovala camasaku, ndipo ana mupasa zina yake Esau. ²⁶ Pambuyo pake mubale wake anacoka, kwanja kwake kunagwira kadenene ka Esau. Anapasiwa zina ya Yakoba. Isaki enze nazaka 60 pamene mkazi wake anabala. ²⁷ Ndipo banyamata banakula, ndipo Esau anakhala oziba kusakira nyama, munthu wa msanga. Koma Yakobo enze munthu wa zii, wamene enze kukhala mumatenthi. ²⁸ Ndipo Isaki anakonda Esau cifukwa anadya nyama zamene anasakira, koma Rabekah anakonda Yakobo. ²⁹ Ndipo yakobo anaphika supu, Esau anabwera kucoka kusanga, analema nanjala. ³⁰ Esau anakamba na Yakobo ati, "Nipaseko supu yofilla napapata nalema!" Ndiye cifukwa zina yake enze Edomu. ³¹ Yakobo anakamba kuti, "Coyamba unigulise ukulu wako," ³² Esau anati ona nili pafupi nokufa, ukulu uli nanchito bwanji kuli ine? ³³ Yakobo anakamba kuti, "Yambira kulumbirira kuli ine" Ndipo Esau analumbila njazi ndipo mnjira iyo anagulisa ukulu waka ku Yakobo. ³⁴ Yakobo anapasa Esau mkate na supu yo phika, ndipo anadya na kumwa, ndipo ananyamuka noyenda. Esau anapepusa ukulu wake munjira iyi.

Chapter 26

¹ Ndipo kunali mu ziko, kumbali kwanjala yoyamba yamene ina chitikka muma siku ya Abrahamu. Isaki anayenda kuli Abimeleki, mfumu yaba Aphistini ku Gela. ² Manje Yehova anaonekela kuli eve naku muuza kuti, "usayende ku Egypito; nkala mu ziko yamene nakuuza kunkala. ³ Nkala mwamene muno mu zika. Ndipo niza nkala naiwe naku kudalisa iwe; kuli iwe naku bobadwa muli iwe, nizakupasa ma ano chamene ninalapila kuli Abrahamu tate wako. ⁴ Nizapakisa bobadwa mwa iwe munga nyenyezi za kumwamba, ndipo nizapasa kuli bobabdwa mwa iwe maziko yonse ayakupitila muli iwe maziko yonse ytapansi yazadalisika. ⁵ Nizachita ichi chifukwa Abrahamu ananvelele mau yanga nakusunga malangizo yanga, lamulo langa, malemba yanga, na malamulo yanga." ⁶ Ndipo Isaki anankala ku Gerari. ⁷ Pamene bazimuna bana funsa pali mukazi wake, anakamba. "Nimulongo wanga." ananvela mantha kukamba, "Nimu kazi wanga," chifukwa enzekuganiza, bazimuna bakuno ku malo bazani paya kuti batenge Rabeka, chifukwa niwabwino." ⁸ Pamene Isaki anakalako maningi kuja Abimeleki mfumu wabo ba Philistini ana sonjela pa (Zenela). Anayanga onani, Isaki anali ku gwila Rabeka, mukazi wake. ⁹ Abimeleki ana muitana Isaki kuli eve ana muza, "Ona, Zoonu nimukazi wako chifukwa nichani unakamba kuti nimu longo wako?" Isaki ana muza eve, "chifukwa nenze kuona munga wina angani paye kuti amu tenge." ¹⁰ Abimeleki anakamba, "Nichani ichi chamena wachita kuli ise? Cinali nichapafupi kuti umozo wabantu agone namukazi wako, ndipo sembe watiletela kuchimwa pali ise." ¹¹ Ndipo Abimeleki anaba Chenjeza bonse bantu naku bauza, "Aliyense wamene azangwila uyu mwamuna olo mukazi wake zoonu azapaiwa." ¹² Isaki anashanga mbeu mu ziko muja naku kolola muchaka chamene kali handredi cifukwa Yehova anamudalisa. ¹³ Anankala mwamuna wolemela, ndipo anankala wolemela ndi kulemela paka anankala wolemela maningi. ¹⁴ Anali na mbelele na ng'ombe zambili nabanja ukulu. Ba Philistini bana mukumbwila. ¹⁵ Manji visime vonse namene banchito batate bake banakumba mumasiku ya Abrahamu tate wake, Ma Philistini bana vilekesa mwaku vifwikala na doti. ¹⁶ Abimeleki anamuza Isaki, "Yenda coka kuli ise, pakuti ndiwe wampavu maningi kuchila ise." ¹⁷ Ndipo Isaki anachokako kuja nakunkala muchifwa ua Gerari, nakunkala mwamene kuja. ¹⁸ Koma futi Isaki anafukulula visime vamanzi, vamene vinakumbiwa mu masiku ya Abrahamu tate wake. Ba Philistini benze bana vifwikila kuchokela pa infa ya Abrahamu. Isaki anavipasa visime ma zina yamene batate bake banali kuvitana. ¹⁹ Pamene banchito ba Isaki banakumba chigwa bana peza kuja cisime chamanzi yoyenda. ²⁰ Bamuna bobeta baku Gerari bana yambana na muna bobeta ba Isaki, ndipo banakamba, "aya nimanzi yatu." ndipo Isaki anaitana cisime "Eseki," cifukwa abayambana nayeve. ²¹ Ndipo bana kumba cisime cinangu, ndipo bana yambana pali icho, futi, ndipo anachitana anachipasa zina "Sitina." ²² Anachoka kuja ndipo anakumba futi cinangu cisime, koma sibana yambana pali ici. ndipo anachitana Tehoboti, nakukamba kuti. "Manje Yehova ati pangila malo ise, ndipo tiza tukuka mu ziko. ²³ Kuchoka apo Isaki anachokako naku yenda ku Beereseba. ²⁴ Yehova anamuokela usiku wamene uja nakukamba, "ndine Mulungu wa Abrahamu tate wako usayope, pakuti nili naiwe ndipo niza kudalisa iwe naku chulukisa bobadwa muli iwe chifukwa cha Abrahamu wa nchito wanga. ²⁵ Isaki anamanga guwa kuja na kuitana pa ziko ya Yehova. Kuja ana kokomela hema, ndipo banchito bake bana kumba cisime. ²⁶ Ndipo Abimeleki anayenda kuli eve kuchokela ku Gerari, na Ahuzzati, na mu zake, na Phico, mukulu wa ba silikali. ²⁷ Isaki anabauza, nichani mwabwelela kuli ine pakuti muni zonda ndipo muna nipisha kuchoka kuli imwe?" ²⁸ Banamuyanka kuti zoonu taona kuti Yehova alina iwe. Ndipo taganiza kuti pankale kulapila pakati patu pakati patu na iwe. Manje tiyeni tipange chipangano naiwe, ²⁹ kuti silizatichita ise choipa, munga mwamene ise sitinaku chite voipa, munga mwamene tinakusungila bwino nakulaila mwa mutendele. Zoonu, ndipo odalisika na Yehova." ³⁰ Ndipo Isaki anabapangila pwando, ndipo bana dya naku mwa. ³¹ Bana uka kuseni maningi naku lumbila kuli wina namu zake. Ndipo Isaki anaba laila, bana musiya mu mtendele. Siku yamene chisime shiba, ndipo zina ya muzinda uja ni Beershiba paka siku yalelo. ³² Siku yamene ija wanchito wa Isaki anabwela naku muuza pali chisime chaene bana kumba. Bana kamba "Tapeza manzi." ³³ Anachitana chisime shiba, ndipo zina ya muzinda uja ni Beershiba paka siku yallelo. ³⁴ Pamene Esau enze na zaka fote, anatenga mukazi, Judi mwana wa Beeri waku Hittiti, naye basimati mukazi wa Eloni waku Hitti. ³⁵ Banaleta misozi kuli Isaki na Rabeka.

Chapter 27

¹ Pamene Isaki anakula na menso yake yanaleka kuonesesa kuti analeka nakuona, anaitana Esau, mwana wake mwamuna mukulu naku mu uza, "Mwana wanga." Esau anati kuli eve "Nili Pano," ² ndipo Isaki anakamba, "Ona kuna nakota siniziba siku yamene nizafa." ³ Chifukwa chaicho tenga zida zako, chola chako cha mivwi, na uta wako, na kuyenda mu sanga nakunigwilila nyama. ⁴ Nipangile chakudya cha bwino, chamene nikonda, ndipo ulete kuli ine kuti nichidye na kuku dalisa iwe nikalibe kufa." ⁵ Ndipo Rabeka anamvela pamene Iski anali ku kamba na Esau mwana wake. Esu anayenda mu sanga kuti agwile nyama nakuleta. ⁶ Rabeka ana uza Yakobo mwana wake mwamuna kuti, "Yangana kuno, namvela atate bako bakamba na mubale waiko Esau. Bakamba kuti, ⁷ 'Niletele nyama yamusanga ndipo unipangile chakudya chabwino, kuti nichidye naku kudatisa iwe pamenso ya Yehova nikalibe kufa.'" ⁸ Ndipo chifukwa chaicho, mwana wanga, mvela mau yanga yamene niku lamula iwe. ⁹ Yenda kuvibeto nakuniletela tubana tw mbuzi tubili twa bwino; ndipo nizatupanga chakudya chabwino cha atate bako, monga mwamene bachikondela. ¹⁰ Uzapeleka kuli atate bako, kuti bachidye nakukudalisa bakalibe kufa." ¹¹ Yakobo anauza Rabeka amai bake, "Onani, Esau mubale wanga ali na upipi, koma ine ndine mwamuna osalala, ¹² kapena batate banga baza ni gwila ine, ndipo nizaoneka kuli beve ngati onama. Nizaziletela tembelelo neka osati daliso." ¹³ Amai bake bana mu uza eve, "Mwana wanga, leka tembelelo ibwele pali ine. Mvelela mau yanga, ndipo yenda, ulete kuli ine." ¹⁴ Ndipo Yakobo anaenda nakutenga tu bana twa mbuzi tubili naku tuleta kuli bamai bake, ndipo bamai bake bana panga chakudya chabwino, monga atate bake banali ku kondela. ¹⁵ Rabeka anatenga vovala va bwino va Esau, mwana wake mukulu mwamuna, wamene anali navo munyumba, naku valika Yakobo, mwana wake mungono mwamuna. ¹⁶ Ana muvalika chikumba cha ka mbuzi kangono ku manja yake na ku mbali yaku mukosi wake osalala. ¹⁷ Anaika chakudya cha bwino na mukate wamene anapanga mu manja mwa mwana wake mwamuna Yakobo. ¹⁸ Yakobo anaenda kuli ba tate bake naku kamba, "Batate banga." Batate bake bana kamba "Nili pano; ndiwe ndani mwana wanga?" ¹⁹ Yakobo ana bauza batate bake, "ndine Esau mwana wanu oyamba. Nachita monga mwenze mwani uzila. Manje ukani nakudyako nyama yanga yamusanga, kutimunidalisa ine." ²⁰ Isaki ana mu uza mwana wake mwamuna, "Nanga wanga?" anati, "Chifukwa Yehova Mulungu wanu aileta kuli ine." ²¹ Isaki anati kuli Yakobo, "Bwela pafupi, pali ine kuti nikugwile iwe, mwana waga mwamuna, kuti nizibe gati zo ona ndiwe mwana wanga Esau olo kapena sindiwe." ²² Yakobo anayenda kuli Isaki tate wake, ndipo Isaki anamugwila naku kamba, "Mau ni mau ya Yakobo koma manja ni manja ya Esau. ²³ Isaki sana muzibe, chifukwa manja yake yenze na upipi, monga ya mubale wake Esau, ndipo Isaki ana mudalisa. ²⁴ Anakamba "Nanga ndiwe zo ona mwana wanga mwamuna Esau?" Anayanka, "Ndiwe" ²⁵ Isaki anti "Leta chakudya kuli ine ndipo nizadya nyama yako yamu sanga, kuti nikudalisa." Yakobo ana muletela chakudya: Isaki anadya, Yakoba anamuletela vinyu, ndipo anamwa. ²⁶ Ndipo atate bake ba isaki bana mu uza. "Manje bwela pafupi nakuni pyopyona mwan wanga mwamuna." ²⁷ yakobo anabwela pafupi naku mupyopyona, ndipo ananusha kafungo ka vovala vake na kumudalisa anakamba "Ona, kafungo kam mwana wanga kali monga kamusanga mwamene Yehova ana dalisa. ²⁸ Mulungu akapase mbali ya mame yako mwamba, mbali yakuina kwa ziko yapansi, na mbeu zambili na vinyu vanyowani. ²⁹ Lekabantu baku sebenzele na maziko yakugwadile unkale bwana kuli ba bale bako, ndipo leka bana bamai bako bamuna baka gwadile iwe uyo wamene azaku tembelela atembelelewe: Wamene azakudalisa adalisiwe." ³⁰ Pamene panja Isaki anasiliza kudalisa yakobo, na yakobo anachoka namata pamenso pa Isaki tate wake Esau mubale wake anabwela kuchokela mukugwila nyama. ³¹ Na eve anapanga chakudya chabwino nakuleta kuli batate bakee. Ana bauza batate bake, "Atate, ukani ndipo mudyeko nyama yamasanga ya mwana wanu, kuti mini dalise." ³² Isaki tate wake anakamba kuli eve, "ndiwe ndani?" anati, "Ndine mwana wanu mwamuna oyamba, Esau." ³³ Isaki ananjenjema maningi nakukamba ati, "Nanga ni ndani wamene enze apaya nyama yamusanga nakuniletela? Ninali nadya yonse ukalibe kubwela, ndipo namudalisa uyo. Zo ona, uyu azankala odalisika." ³⁴ Pamene Esau anamvela mau ya atate bake, analila maningi, mokalipa naku kamba kuti kuli batate bake, "Nidaliseni ine, naine batate banga." ³⁵ Isaki anakamba, "Mubale wako enze abwela kuno monamiza, nakutenga madaliso yako." ³⁶ Esau anakamba, "Uyu zoonza zina yake si yakobo chifukwa aninama ine kabili anaipoka choyenela chaku badwa kwanga, ndipo, onani, manje atenga madaliso yanga. Ndipo anakamba, "Simunanisugileko daliso?" ³⁷ Isaki anayaka naku kamba kuli Esau, "Ona, namupanga bwana wako, nakumupasa babale bake bonse monga ba nchito, ndipo na mupasa mbeu na vinyu ya sopano. Nanga nichani chamene ningakuchitila, mwana wanga mwamuna?" ³⁸ Esau anakamba kuli batate bake, "Mulibe olo daliso imozi yanga, atate banga? Ni daliseni, naine, atate banga." Esau analila mo punda. ³⁹ Isaki atate bake banayanka nakukamba kuli eve, "Ona, malo kwamene uzayenda kunkala yaza nkala ku tali na chuma cha ziko yapansi kutali na mame yakumwamba. ⁴⁰ Kupitila mulupanga yako uzankala, naku sebenzela mubale wako. Koma ngati wamu ukila, uzachosa goli yake mu mukosi wako." ⁴¹ Esau anamuzonda yakobo chifukwa cha

madaliso yamene bana mupasa batate bake. Esau anakamba mumutima wake, "Masiku yolila batate banga yali pafupi; yakapita nizamupaya mubale wanga Yakobo." ⁴² Mau ya Esu mwana mwamuna yana uziwa kuli Labeka. Ndipo anaitana Yakobo mwana wake mwamuna mungono naku kamba kuli eve, "Ona Esau azitontoza eka pali iwe pakuganiza ku kupaya iwe. ⁴³ Manje, mwana wanga mwamuna, nimvelele ine nakutabila kuli Labani, mubale wanga, mu Halani, ⁴⁴ Kankaleko na eve pangono, mpaka ukali wa mubale wako uchepeko, ⁴⁵ mpaka ukali wamubale wako uchokeko kuli iwe, nakuibala vamene una chita kuli eve. Ndipo nizatuma nakuku bweza kuno. Nichifukwa cha chani niza kutayani bonse babili pa siku imozi? ⁴⁶ Rabeka anakamba kuli Isaki, "Nalema nao umoyo chifukwa cha bana bakazi baku Heti ngati yakobo akwatila bana bakazi bena bana bakazi bakuno kumalo, umoyo wanga uzankala bwino bwnji?"

Chapter 28

¹ Isaki anaitana Yakobo, anamu dalisa, nakumulamulila, "usaka tenge mukazi ochokela kuli bazikazi baku Kenani. ² Nyamuka, yenda ku Padani Aramu, ku nyumba ya Bethueli ba mai ba batate bako naku tenga mukazi kuchoka kuja, umozi mwana mukazi wa Labani, mubale wa bamai bako. ³ Leka Mulungu wampamvu zonse aku dalise, aku pange obala ndipo akuchuluse kuti munkale bantu bambili. ⁴ Leka akupase daliso ya Abrahamu, kuli iwe, naku bana bobadwa pambuyo pako kuti ungene muziko yamene unali kunkalamo, yamene Mulungu anapasa Abrahamu." ⁵ Pamene apo Isaki anatuma Yakobo. Yakobo anayenda ku Padani Aramu, kuli Laban mwana mwamuna wa Betulo waku Aramea mubale wa Rebekah, ba mai ba Yakobo na Esau. ⁶ Manje Esau anaona kuti Isaki anadalisa Yakobo na kumutuma kuyenda ku Padani Aramu, kuti akatenge mukazi wa kuja. Anaona futi, kuti Isaaki anamudalisa na kumulamulila kuti, "usaka tenge mukazi pa bakazi baku Kenani." ⁷ Esau anaona futi Yakobo anamvelela batate bake naba mai bake, nakuyenda ku Padani Aramu. ⁸ Esau anaona kuti bakazi baku Kenani sibana kondwelese batate bake. ⁹ Pamene apo anayenda ku Ishmaeli, nakutenga, kumbali kwa bakazi bake, Mahalati mwana mukazi wa Ishmaeli, mwana mwamuna wa Abrahamu mulongosi wa Nebaioti, ankale mukazi wake. ¹⁰ Yakobo anachoka ku Beersheba naku yenda caku Harani. ¹¹ Anabwela pa malo yena naku nkala kuja usiku onse, chifukwa zuba yenze inangena. Anatenga mwala umozi mu malo muja, naku ika pansu pa mutu wake, naku gona pa malo paja. ¹² Analota naku ona makwelelo yana ima kuchoa pa ziko yapansi. Pamwamba pake panafika kumwamba ndipo bangelo ba Mulungu benzeli ku kwelapo naku selukapo. ¹³ Onani, Yehova anaimilila pamwamba pake naku kamba, "Ndine Yehova, Mulungu wa Isaki. Pa malo yamene ya gona nizapasa iwe na bana bobadwa muli iwe. ¹⁴ Bana bobadwa muli iwe bazankala monga doit yapansi, ndip muza zulana mutali wa kumazulo, kumawa, kumpoto, ndipo na kumwela, kupitlila muli iwe namuli bobadwila muli, mabanja yonse yapa ziko yaza dalisika. ¹⁵ Onani, Nili na iwe ndipo nizaku sunga kuli konse kwamene uzaka yenda. Nizakuleta iwe mu malo aya nafuti: chifukwa sisizaka kusiya niza chita vonse vamene nina lonjeza kuli iwe." ¹⁶ Yakobo ana uka mutulo mwake, ndipo anakmba, "zo'ona Yehova ali pano pamalo, koma sininazibe. ¹⁷ Anali na manta naku kamba, "Niyo yoyofya bwanji aya malo! aya siyena koma nyummba ya Mulungu. Apa nipolobeka kumwamba." ¹⁸ Yakobo anauka kuseni maningi naku tenga mwala wamene anabwela afaka pasni pa mutu wake. Anachipanga nga chipilala naku tilapo mafuta pamwamba pake. ¹⁹ Anaitana zina malo yaja Betheli, koma zina ya muzinda uja inali Luzi. ²⁰ Yakobo analapa chilapilo, kuti, "Ngati Mulungu azankala naine na kuni chigiliza pa njila iyi pamene niyenda, na kunipasa mukate okudya, na vovala vovala, ²¹ chakuti ine nibwelele mwamu tendele ku nyumba ya batate banga, pamene Yehova azankala Mulungu wanga. ²² Pamene mwala yuy wamene na imilika ngati pilala uzankala opatulika kuchokela pali vonse vamene wani pasa nizabwelesa chakumi kuli iwe."

Chapter 29

¹ Pamene apo Yakobo anayenda paulendo wake na kufika ku malo ya bantu ba ku maba. ² Pamene anayangana, anaona chisime mumunda, na, onani, magulu yatatu ya mbelele yanali gone mumbali. chifukwa cikuchoka mu chicime ichi banali kumwesalamo mbelele, na mwala unali pakamwa pachisime unali ukulu. ³ Pamene yonse magulu mbelele yanakumana paja, na bachibeta banali kuchosa mwala pakamwa pachisime na kupasa mbelele manzi, naku bwezapo chimwala futi pakamw pachisime, nakuchibweza mumalo yake. ⁴ Yakobo anakamba kuli benve kuti, "ba bale banga, mwachokela kuti?" bana yanka, "Tachokela ku Haran." Anakamba kuli benve, ⁵ "Mumuziba Labani mwana mwamuna wa Naha? "Nabenve banakamba kuti, "Timuziba." ⁶ anakamba kuli benve kuti, "mwati alibwino?" Benve banakamba kuti, " alichabe bwino, na, yangananei kuja, Recho mwana wake mukazi abwela na mbelele." ⁷ Yakobo anakamba, "Onani, ni pakati pa siku. sintawi yama guli ya mbelele kukumana pamozi. mufunika kupasa mbelele manzi na kuyenda na kuzileka zidye." ⁸ Banakamba kuti, "sitinga zipase manzi mpaka zonse mbelele zikumane pamozi. Na bamuna baza chosa chimwala pachisime kuchoka apo tizazipasa manzi mbelele." ⁹ Pamene Yakobo anali kukamba na benve, Recho ana bwela na mbelele zaba tate bake, chifukwa niwamene anali kuzibetela. ¹⁰ Pamene Yakobo anaona recho, mwana mukazi wa Labani, mubale wa bamai bake, na mbelele za Labani, mubale wa bamai bake, Yakobo ana bwela pamene paja, naku vendesa mwala kuchoka pakamwa pachisimenakupasa manzi gulu ya mbelele za Labani, mubale wa bamai bake. ¹¹ Yakobo ana pyopyonta Recho nakulila mo kuwa. Yakobo anauza Recho, kuti enve anali bululu wa batate bake, anali mwana wa Rabeka. ¹² Pamene apo enve anatmnaga na kuyenda ku'uza batate bake. ¹³ Pamene Labani ananvela iyi nkani ya Yakobo mwana mwamuna wamulonosi wake, anamanga kuti bakumane na enve, na kumukumbatila, na kumu pyopyonta, na kumu bwelesa ku nyumba yake. Yakobo anauza Labani vonse ivi vintu. ¹⁴ Labani ana kamba kuli enve, "iwe zo'ona ndiwe fupa yanga na munofu wanga." ndiye pamene Yakobo ana nkala na paka ntawi ya mwezi umozi. ¹⁵ Ndiye pamene Labani anakamba kuli Yakobo kuti unga ni sebenzele mahala chifukwa ndiwe bululu wanga? Niuze, malipilo yako yazankala bwanji?" ¹⁶ Manje Labani enzeli na bana bakazi bali. Na zina ya mukulu yenze Leya, na zina ya mungono yenze Recho. ¹⁷ Menso ya Leya yanali yofewa, koma Recho anali okongola, mukapangidwa nama onekedwe. ¹⁸ Yakobo anakonda Recho, ndiye chamene anakambila, "nizaku sebenzelani zaka seveni ya Recho, mwana wanu mun'gono mukazi. ¹⁹ Labani anakamba kuti, "nicha bwino kuti ine nipupase enve kuli iwe, osati ine nipase enve kuli mwamuna wina. nkala na ine." ²⁰ Na Yakobo anasebenza zaka seveni ya Recho; koma yanamuonekela kwati nimasiku yangono, chifukwa cha mwanen ana mukondela. ²¹ Pamene apo Yakobo anakamba kuli Labani, "nipase ine mukazi wanga, chifukwa masiku yanga yakwanila kuti nimukwatile!" ²² Manje Labani anaitana pamozi bantu bonse ba pamalo nokupanga pwando. ²³ ²⁴ ²⁵ Mumazulo, Labani anatenga Leya mwana wake mukazi nakumubwelesa enve kuli Yakobo, wamene anangena muli enve. Labani anapasa wanchinto mukzai Zilpankuli mwana wake mukazi Leya, kunkala wanchonto ake. Kuseni, onani, enze Leya! Yakobo anakamba kuli Labani, "nanga ndiye vichani vamene wa chita kuli ine? nanga ine sinina sebenzele Recho? Nichifukwa cha chani mwani nama ine?" ²⁶ Labani anakamba, simwambo watu kupasa mwana mukazi mungono tikalibe kupasa mwana mukulu. ²⁷ Silizisa mulingu wa uy mwana mukazi, koma tizakupsa na winangu munga malipilo pakuni sebenzela zaka seveni zinangu." ²⁸ Yakobo anachita sochabe, naku siliza mulingu wa Leya. Ndiye pamene Labani anamupasa Recho mwana wake mukazi kunkala mukazi wake an enve. ²⁹ Labani ana pasa Bilhah kuli mwana wake mukazi Recho, kunkala wanchito wake. ³⁰ Na Yakobo anangena muli Recho, na enve, koma ana konda Recho kupambana na Leya. Na Yakobo anamusebenzela Labani zaka zinangu zili seveni. ³¹ ³² Yehova anaona kuti Leya sanali okondewa, anasegula mala yake, koma Rcho analibe mwana. Leya anankala namimba nakubala mwana mwamuna, nakumu itana ina Rubeni. chifukwa anakamba kuti, "Chifukwa Yehova ayangana paku vutika kwanga; zo'ona apa maje bamuna banga bazani konda ine. ³³ Ndiipo anakahala namimba futi na kubala mwana mwamuna. Ana kamba, "Chifukwa Yehova anvela kuti sindine okndewa, anipasa futi mwana mwamuna."Ana mupasa zina Simioni. ³⁴ Anankhala futi namimba nakubala mwana mwamusa. Anakamba, "apa manje bamuna banga bazangwilikana kuli naine, chifukwa naba balila bana bamuna batatu."Chaicho anaitaniwa zina ya Levi. ³⁵ Ankhala na mimba futi nakubala mwana mwamuna anakamba, "ino ntawi nizamutamanda Yehova. Ndiye pamene apo ana mu itana zina yake Yuda; ndipo analaka kunkala na bana.

Chapter 30

¹ Pamene Recho anaona kuti sana mubalile bana Yakobo, Recho anakumbwila mulongosi wake. Anakamba kuli Yakobo kuti, "Nipase bana, olo inzafa." ² Yakobo anakalipa chifukwa cha Recho. Anakamba kuti, "Ushe Ndine mulungu, anakulesa kuti unkale nabana?" ³ Anakamba kuti, "Ona, Pali wanchito wanga Bila. Gona naye, chakuti ati balile bana bolela pa mendo panga, ndipo ine nizankala na bana kupitila muli enve." ⁴ Chakuti anamupasa Bila wanchito wake kuti ankale mukazi wake, ndipo Yakobo aanagona naye. ⁵ Bila anankala na mimba nakubala mwana mwamuna wa Yakobo. ⁶ Pamene apo Recho anakamba kuti, "Mulungu anikambilako, ndipo anvela na mau yanga nakunipasa mwana mwamuna." Chifukwa chaichi anamuitana zina yake yake Dani. ⁷ Bila, wanchito wa Recho, anankala namimba futi naku balalila Yakobo mwana mwamuna wachibili. ⁸ Recho anakamba kuti, "Namenyana na mulongosi wanga mwampavu ndipo napambana." Anamuitana zina yake Nafutali. ⁹ Pamene Leya anaona kuti aleka kubala bana, anatenga Zelipa wanchito wake nakumupasa kuli Yakobo kuti ankale mukazi wake. ¹⁰ Zelipa, wanchito wa Leya, anabalila Yakobo mwana mwamuna. ¹¹ Leya anakamba kuti, "Uyu ndiye mwayi!" chakuti anamuitana zina yake Gadi. ¹² Pamene Zelipa, wanchito wa Leya, anabalila Yakobo mwana mwamuna wachibili. ¹³ Leya anakamba kuti, "Nakondwela! Chifukwa bana bakazi bazani itana ine kuti okondwela." Chakuti anamu itana zina yake Asha. ¹⁴ Rubeni anayenda mu munda pa masiku yochosa witi nakupeza maudeleki mu munda. Anayabwelesa kuli mayi wake Leya. Pamene Recho anakamba kuli Leya, "Unipaseko maudeleki yenangu ya mwana wako mwamuna." ¹⁵ Leya anakamba kuli enve, "Iyi ninkani ing'ono kuli iwe? kuti unanipoka mwamuna wanga? Manje ufuna kunitengela na mandeleki ya mwana mwanga mwamuna?" Recho anakamba kuti ndiye pamene azagona naiwe usiku walelo, chifukwa cha mandeleki yamwana wako yamene uzani pasako mochinjanisha." ¹⁶ Yakobo anabwela kuchokela kumunda mumazulo. Leya anayenda kukumana naye nakukamba kuti, "Ufunika kugona na ine, chifukwa nakugula na mandeleki." Chakuti Yakobo anagona na Leya usiku. ¹⁷ Mulungu anamunvelela Leya, anankala na mimba nakubalila Yakobo mwana mwamuna wa nambala faivi. ¹⁸ Leya anakamba kuti, "Mulungu anipasa ine malipilo yanga, chifukwa namupasa muzimai wanchito wanga kuli bamuna banga." Anamupasa zina yake Isaka. ¹⁹ Leya anankala namimba nakubala mwana mwamuna wa nambala sikisi wa Yakobo. ²⁰ Leya anakamba kuti, "Mulungu anipasa ine mpaso yabwino. Apa manje mwamuna wanga azani lemekeza ine, ndaba namubalila bana bamuna bali sikisi." ²¹ Pasogolo pake anabala mwana mukazi nakumupasa zina yake Dinna. ²² Mulungu anakamba na Recho mumaganizo naku munvelela. ²³ Anamulengesa kuti ankale na mimba. Anankala na mimba nakunkala na mwana mwamuna. Anakamba kuti "Mulungu anichosa nsoni zanga." ²⁴ Anamuitana zina yake Yosefe, kukamba, kuti, "Yawe alundilapo kuli ine mwana mwamuna winangu." ²⁵ Pasogolo pake Recho anabala Yosefe, "Yakobo anakamba kulli Labani "Munimasule, pakuti niyenfe kumunzi kwatu nako ziko yanga. ²⁶ Munipase bakazi banga na bana banga bamene ninalipilila malipilo yokugwililani nchito, futi munileke niyende, kainge muziwa bwino nchito yamene nakugwili lani." ²⁷ Labani anamu uza kuti, "Ngati apa uzani chitila chifundo mwamene uvionela vintu, uyembekeze, chifukwa nina ziba mumatesnga kuti Yawe anidalisa ine chifukwa cha iwe." ²⁸ Pamene apo anakamba kuti, "kamba mutengo wako weka, ndipo ine nizabalipila." ²⁹ Yakobo anakamba kuli enve, "Uziba mwamene ninatumikila kuli iwe, na mwamene vinyama vako vachitila twino kuli ine. ³⁰ Pakuti mwenze natungo'no pamene ine nikalibe kubwela manje vapakilapo maningi. Yawe anakudalisani imwe paliponse peninali kusebenzela. Nanga niliti pamene nizapasako wamunyumba mwanga naine?" ³¹ Labani anafunsa kuti, "Nizakulipila chani?" Yakobo anakamba kuti "Simuzanilipila chilichonse. Ngati munga nichitele ichi chintu kuli ine, nizakavidyesa futi vinyama vanu nakusamala. ³² Lekani ine nipitemo pakati pa vinyama vanu lelo nakuchosapo ka shipi kalikonse kamene kali nama iwanga natuma dontho, ndipo kabulaki pa mbelele, ndipo katuma dontho namizele pagulu ya mbuzi. Aaya ndiye yazankala malipilo yanga. ³³ Kukulupilika kwanga kuzakanikambilako pasogolo panga, mukayende kuona malipilo yanga. Iliyonse yamene siyizankala na mizele na madoti pakati pa mbuzi, nayo kuda pakati pa mbelele, ngati iliyonse izakapezeka naine, izakaganizilidwa kuti niyakuba," ³⁴ Laban anakamba kuti, "Anavomela. Leka mwamene wakambila mau yako." ³⁵ Yamene ija siku Labani anachosapo mbuzi zimuna zamene zenzeli na mizele na madoti, na mbuzi zikazi zonse zamene zenze naka wayiti pa tupi, na zonse zokuda pakati pa mbelele, nakuzipasa mumanja mwa bana bake bamuna. ³⁶ Labani anayikapo ulendo wamasiku yatatu pakati payenve mwine na Yakobo. Chakuti Yakobo anapititliza kusebenza kusunga vinyama va Labani vamene vina salapo. ³⁷ Yakobo anatenga misambo yafuleshi yojubiwa yawisi ya mtengo wapopula, na mutengo wa alamondi, na mutengo wapuleni, naku fundulamo tumilayeni twa waiti mpaka va wayiti vamukati mwa chimutengo vinaonekela ku tumi tengu. ³⁸ Pamene apo anayika tumitengo twamene anafundula pasogolo pa vinyama, pasogolo pama kontena yomweselamo manzi vinyama, pamene vinali kubwela kumwa manzi vinyama vinankala nama mimba pamene vinabwela kumwa manzi. ³⁹ Vinyama

vinali kugonana pafupi na tumitengo; ndipo vinyama vinabala bana bamizele, bamawanga na madoti.⁴⁰ Yakobo anapatulapo mutundu yuy wa tubana twa mbelele, koma analeka kuti zonse zinangu ziyangane ksayidi kwe kunali vinayama vamizela vo kuda pavinyama va Labani. Pasogolo pake anazichoselapo vinyama vake mwine yeka ndipo sanali kusankaniza pamozi na vinyama va Labani.⁴¹ Paliponse nkosa zolimba muvinyana zikayamba kugonana. ninshi Yakobo analikugoneka tumitengo mumakontena yomwelesamo manzi vinyama, apo vinyama vilangana patumitengo.⁴² Koma pamene vinyama vo foka maningi vinabwela, sanayike tumitengo pafupi navo. Chakuti vinyama vofoka vinankala va Labani, ndipo volimba vinankala va Yakobo.⁴³ Mwamuna yuy anankala olemela maningi. Anali na vinyama vambili, wanchito bakazi na bamuna, makameleo nama donke.

Chapter 31

¹ Ndipo Yakobo anamva mau ya bana ba Labani, yamene banakamba, "Yakobo atenga vonse va batate bathu, apeza chuma conse ici kuckela mu vinthu va batate. ² Yacobo anaona kayang'anidwe pa menso pa Laban. Anaona kayang'anidwe kake kanacinja. ³ Ndipo anatuma ndi kuitana Rakele ndi bwelala kuziko ya batate bako na ba bale bako ndipo nizankhala naiwe. ⁴ Yacobo anatuma ndi kuitana Rakele ndi Leya kui abwele kumunda kuli zobeta zake. ⁵ Ndipo anakamba na beve, "Naona kayanganidwe kaba tate banu pali ine kacinja, koma Mulungu wa tate ali naine. ⁶ Muziba kuti na mpavu zanga zonse nankhala nisebenzela batate banu. ⁷ Batate banu baninama na kucinja malipilo yanga kali 10, koma Mulungu sana muvomeka kucita coipa. ⁸ Ngati anakamba kuti, nyama za manthongo ndiye malipiro yako, 'ndipo zonse nyama zinabala zamanthongo, ngati akamba kuti, zamizela zizakhala malipiro yako, 'ndipo nyama zonse zinabala zamizera. ⁹ Cifukwa cake Mulungu anatenga nyama za batate banu na ni pasa. ¹⁰ ndipo pa nthawi yobala, ninaona muciloto mbuzi zimuna zinali kukwela nyama. Mbuzi zimuna zinali namizela, na mamphongo na mitundu yosiyana-siyana. ¹¹ Mungelo wa Mulungu anakamba na ine mu ciloto, 'Yakobo' ninakamba, 'nili pano.' ¹² Anakamba kuti, nyamula menso yako ndipo uone mbuzi zonse zimuna zikwelana na nyama. Zinamizela mamphongo, na mitundu yosina-siyana, cifukwa naona vonse vamene Labani acita kuli iwe. Ndine ¹³ Mulungu wa Betele, kwamene unathila mafuta pamwala, kwamene unalumbila kuli ine. Manje nyamuka ucoke m'malo yano na kubwelela kumalo kwamene unabdwila." ¹⁴ Rakele na Leya anayankha na kukamba na eve, nanga kulibe mbali na vosalila vathu munyumba ya batate? ¹⁵ Sitisungiwa na eve monga ni balendo?cifukwa atigulisa nakuonongeltu nadalama zathu. ¹⁶ Pa cuma ciliconse camene bacosako kuli batate bathu cankhala cathu na bana bathu. Manje, vilivonse vamene Mulungu akamba, cita." ¹⁷ Ndipo Yakobo ananyamuka noika bana bake bamuna na bazikazi bake pa ma bulu. ¹⁸ Anaika zobeta zake pa songolo pake, pamozi nakatundu wake bonse, kuikilapo nanyama za mene anakhala nazo mu paddani Aramu. Ndipo anakonzekera kuyenda kuli Isaki tate wake mumalo yao ya Kanaani. ¹⁹ Pamene Labani anayenda kukasenga nkhusa zake, Rakele anaba tumilungu twa munyuma ya batate bake. ²⁰ Yakobo ana namanso Labani wa ku Aramean, po samu uza ati ayenda. ²¹ Ndipo anathaba na vonse enze navo na kudusa pa mumana, ndipo anayendela ku phili yaziko ku Giliyadi. ²² Pasiku ya citatu Labani ana uziwa kuti Yakobo anathaba. ²³ Ndipo anatenga abale ake ndi kumupisha kwa ulendo wamasiku seveni. Anamupeza pa phiri ya ziko ya ku Giliyadi. ²⁴ Ndipo Mulungu anabwera kwa Labala mu Aramean muciloto naku mu uza kuti, "Nkhala ocenjera kuti osakambe voipa olo vabwino kuli Yakobo. ²⁵ "Labani anapitilila Yakobo. Ndipo Yakobo anamanga hema yake mupili yaziko. Labani naye anakhala paja mba bale bake mupili ya Giliyadi. ²⁶ Ndipo Labani anakamba kuli Yakobo, wacita cani, kuti unani nama nakunyamula bana banga bakazi monga ba kaida ba nkondo? ²⁷ Cifukwa nicani unathaba mwacisinsi na kuninama ndiponso sunani uze ine? Asembe nina kupelekeza nakusangalala na nyimbo, ndi lingaka ndi coliza. ²⁸ Sunandi vomekeze ine ku mpsompsona bana banga bakazi na bamuna, manje wacita vopusa. ²⁹ Vili mu mphavu zanga kukucita voipa, koma Mulungu waba tate bako anakamba usiku wasila ndipo anati, 'Khala wocenjela, kuti osakambe kuli Yakobo voipa na vabwino.' ³⁰ Manje wayenda cifukwa wenze kufuna maningi kubwelela kunyumba ya batate bako. Nanga nichani camene unabela milungu yanga?" ³¹ Yakobo anayankha nanena kwa Labani, "Chifukwa ninayopa nakuganiza kuti muzapoka bana banu bakazi mwampavu ndaba sinilaile. ³² Alionse wamene aba milungu yanu saza pitiliza kukhala na moyo. Pamenso ya ba bale bathu, ona cili conse cili naise ngati nichanu mucitenge. "Cifukwa Yakobo sanazibe kuti Rakele ndiye anaba. ³³ Labani anangena muhema ya Yakobo, na muhema ya Leya, ndiponso muhema ya banchito babili, koma sanaba peza. Anocoka muhema ya Leya na ku ngena muhema ya Rakele. ³⁴ Ndipo Rakele anali anatenga milungu zamunyumba, anaviika pa conkhalila caca ngamila, ndi kunkhalapo. Labani anasakila muhema yonse, koma sana vipeza. ³⁵ Anakamba kuli atate bake, "Osakalipa, mbuye wanga, kuti siningamilile pamenso pano, cifukwwa nili panthawi ya kumwezi. "Ndipo anasakila koma sana peza milungu za munyumaba mwake. ³⁶ Yakobo anakalipa naku kangana na Labani. Anakamba kwa iye, "Kodi mulandu wanga ndiwa bwanji?Cimo yanga niya bwanji, kuti muzingo kuni konka konka? ³⁷ Popeza mwa sukila ponge pali katundu yanga. Nichani came mwapeza pavinthu vonse va munyumba yanu? Vileteni apa pali abale athu, kuti ba weruzu pakati ka ife. ³⁸ Kwazakatwenti na nkhalala naimwe. Nkhosa zanu nambuzi zikazi sizina kangangapo kubala, olo kapena kudyapo pa vo beta vako. ³⁹ Vina vina ng,ambiwa na vilombo sinina vilete kuli iwe, koma, ndine ninalipila pava mene vinasowa. Nthawi zonse mumanindi pilisa pali nyama yadoba, loko yabewa usiku olo muzuba. ⁴⁰ Ndipo nenzeko, musiku zuba inani shoka, mame ya usiku ndipo sinina gone usiku. ⁴¹ Izi zake twenti nankhala munyumba yako, nina kusebenzela iwe zaka fotini cifukwa ca bana bako babili bakazi, nazaka sikisi vobeta vako. Mwacinja malipilo kali teni. ⁴² Pokhapo Mulungu wa batate banga, Mulungu wa Abrahamu ndi iye wamene kaki ayopa, anali na ine, zo ona mwenze kuti niyende popanda vilivonse mu manja mwanga. Mulungu ayangana kuvutika

kwanga na mwamene nenze kusebenzera maningi, ndipo anaku kalipila busiku wayenda." ⁴³ Labani anayankha na ku kamba kuli Yakobo, "Akazi aba ndiye bana banga bakazi, bazukulu niba zukulu bangaa, navobeta ni vobeta vanga. vonse vamene uona nivanga. Koma nichani lelo ninga cite kuli aba banga bakazi kapene bana bao bamene bana bala?" ⁴⁴ Manje apa, tiye tipange cipangano, iwe naine, ndipo ndiye ciza nkhalamboni pakati ka iwe na ine." ⁴⁵ Ndipo Yakobo anatenga mwala nakuika pamwamba pa pila. ⁴⁶ Yakobo anakamba kuli babale bake, "Ikani miyala pamozi," ndipo banatenga miyala nakuzi bunjika. Ndipo banadyela pamwamba. ⁴⁷ Labani ana itanapo Jegara saha Duthu, koma Yakobo anaitanapo Gilayadi. ⁴⁸ Labani anakamba, izi miyala ni kamboni pakati kaiwe naine, lelo "Cifukwa cake zina yake baitanapo Giliyadi. ⁴⁹ Paitaniwanso mizipa cifukwa Labani anakamba, Leka Yehova ayangane pakati kaiwe na ine, pamene tisiyana wina na muzake. ⁵⁰ Ngati suzasunga bana banga bakazi bwino, olo uzatenga bakazi bena pambali ya bana banga bakazi, loko palibe wina ali naise, ona, Mulungu ni kamboni pakati kaiwe na ine." ⁵¹ Labani anakamba kuli Yakobo, "Yangana pamwamba, ndipo ona pa pila, yamene naika pakati kaiwe naine. ⁵² Iyi nthutu ndiye kamboni, na pila ni kamboni kuti sinaza jumpa iyi nthutu kubwera kuli iwe, ndipo na iwe suza jumpa iyi nthutu ku bwela kuli ine, kucita voipa. ⁵³ Leka Mulungu wa Abrahamu, na Mulungu wa Nahor, na milungu za ba tate bao, ziweruza pakati kathu." Ndipo Yakobo analapa pakuyopa batate bake Isaki. ⁵⁴ Yakobo ana peleka nsembe pa phiri nakuitana abale bake kuti bazadye cakudya. Ba nadya na kunkhala busiku bonse pamwamba pa lupili. ⁵⁵ mumawa, Labani anauka, naku myompyona bazulu bake na bana bake bakazi na kubadalisa. Pamene Labani anacokapo nakubwelera kunyumba.

Chapter 32

¹ Naye Yakobo anayenda njila yake naba ngelo ba Mulungu bana mukumanya iye. ² Pamene Yakobo ana one, "anakamba iyi i hema ya Mulungu." ana itana zina yayaja malo mahanayimu. ³ Yakobo ana tuma atumikila kusogolo kwake kuli mubale wake Esau mumalo yaseya, mu malo ya Edomu. ⁴ Anabalamulila kukamba, Izi ndiye zamene uzakamba kuli mbuye wanga Esau. Ichi ndiye chamena akamba Yakobo kapolo kwanga kufika lelo. ⁵ Nili ng' ombe na abuvu. na vaweta naba nchito bamuna na bakazi. Natuma aya mau kuli abwna banga kuti apeze mwai mu menso yako. ⁶ A mithenga banabwela kwa Yakobo ndipo anati, "Tina yenda kuona mubale wako Esau. Abwela kuzakumana naiwe, nabamuna bali fihandredi bali nayeve. ⁷ Ndipo Yakobo anayopa na kukwiya. Ndipo anagaba banthu bamene enze mumagulu yabili, na vobetaa, ng' ombe, ndi mabulu. ⁸ Anakamba kuti, "Ngati Esau abwela kugulu imozi ndi kuimenya, ndipo gulu yamene izasala izathaba. ⁹ yakobo anati, "Mulungu wa atate banga Abrahamu, ndi Mulungu wa batate banga Isaki, Yehova anakamba kwa ine, Bwelela ku ziko lako ndi kwa abale ako ndiponizakupeleka pasongolo. ¹⁰ Sindine oyenela pali vonse vocita vacipangano co kholulupilila ndi zabwino ¹¹ Napapata ni pulumuseni ku kwanja yu mu bale wanga, ku kwanja kwa Esau, chifukwa nili na mantha kuti azabwele ndi kundimenya ndi bazimai nabana. ¹² Koma wakamba kuti, "Nizakupanga kuti utukuke nizapanga bana bako monga dohti ya munyanja, yamene singabelengeke mu ma nambala. ¹³ Yakobo anakhamba uja usiku uja. Anatenga vina enze navo monga mphaso kuli Esau, mubale wake. ¹⁴ Mbuzi zikazi zili thu handiledi ndi mbuzi zimuna zili twenti, nkhusa zikazi zili thuhandiledi, ndi nkhusa zimuna twenti. ¹⁵ Ngamila zamkaka zili feti na tu bana twao. Ng'ombe zikazi zili fote, na ng'ombe zimuna zili teni, mabulu yakazi yali twenti ndi ma bulu yamuna yali tenni. ¹⁶ Ivi anapasa mumanja nwa ba nchito bake, gulu payekha yeke, anakamba kuli ba nchito, "Pitani kusogolo kwanga ndipo muike mupata pakati panagulu. ¹⁷ Aba uza wa nchito woyamba kuti, pamene Esau mubale wanga akumana naiwe na kukufunsa, kukamba, ili kumbali yandani? Upita kuti? ni nyama zandani izi zili kusogolo kwako? ¹⁸ Ndipo uza kamba kuti, 'ndiwa nchito wako Yakobo ndi mphaso yatumi ziwa kuli bwana wanga Esau. Ona, naye alikubwela mumbuyo mwathu. ¹⁹ Yakobo anapasanso malamulo gulu lacibili, lacityatu, ndi amuna onse ana konka, ng' ombe. Anakamba, muzakamba vinthu vimozi mu kakumana ndu Esau. ²⁰ Mufunika kukamba wa nchito wako Yakobo abwela pambuyo, "Cifukwa anaganiza," nizamu kondwelesa iye na mphaso zamene nituma kusogolo kwanga pambuyo pake, nikamu ona paena azandi landila ine. ²¹ Mphaso zina yendelatu ku sogolo kwake. Iye usiku uja anakhala mu hema. ²² Yakobo anauka usiku ndipo anatenga bakazi bake babili, banchito bake babili bazimai, nabana bake bamuna levini, anabatuma kutauka pa abokola Yabboki. ²³ Munjila iye anabatuma kutauka mumana na cuma cao conse. ²⁴ Taboko anasijiwa yeka, ndipo analimbana na munthu pakana kunaca. ²⁵ Pamene uja munthu anaona kuti sinizamkwanisa, anaonga nchafuyake, nchafu ya Yakobo inasinthani pamene banali kulimbana. ²⁶ Munthu uja anakamba, nisiye, apeza kwayamba kucha, "Yakobo anakamba, "Sinizakuleka pakana unidalise. ²⁷ Munthu anakamba kuli yeve, "Zina yako ndiwe ndani? Yakobo anati, "Yakobo." ²⁸ Munthu anakamba, zina yako sizikhlnso Yakobo koma Israeli. Chifukwa walimbana ndi Mulungu ndi banthu koma wa pambana. ²⁹ yakobo anafunsa, "Napapata niuze zina yako? Anati, "Ufunsila chani zina yanga? ndipo anamusalisa paja. ³⁰ Yakobo anaitana pamalo paja kuti peniwenlo popeza anti, naona Mulungu menso na menso ndipo moyo wanga wapulumuka. ³¹ Zuba inacoka pamena Yakobo anadusa peniwelo anali ku golontha chifukwa ca achafu yake. ³² Ndiye chifukwa cake kufika nalelo banthu ba ku israeli si kudya nyama zamene zipezeka pafupi nanchafu cifukwa munthu ana onanga zibalo pa ku siyanisa nchafu Yakobo.

Chapter 33

¹ Yakobo onayangana kumwamba, onani, Esau akubwela, pamodzi naive anali amuna ake 400. Yakobo anabagawa bana bake pakati pa ba leya, ba rakele ndi anchito akazi abili. ² Ndipo anaika anchito na bana bawo kiutsogolo, kukonkapo anali leya na bana bake na kukonkapo anali Rakele na Yosefe kumbuyo kwa bonse. ³ Iye mwine anayenda patsogolo pa bonse. Iye anagwanda pansi ka 7, kufikila anafika pafupi na mbale wake. ⁴ Esau anamutamangila iye, na kumukumatila, na kumulandila ndi kumufyofyonta. Ndipo iwo analila. ⁵ pamene Esau anayangana ku sogolo, anaona azimai ndi bana. Iye anakamba, " Nindani awa banthu amene bali na iwe? " Yakobo anakamba, " Aba ni bana amene Mulungu mwacisomo cake anapasiwa na wancito wanu." ⁶ Ndipo banchito akazi banafika pamodzi ndi bana bawo ndipo banagwanda pansi. ⁷ Wokonkhapo anali Leya ndi bana bake anafika ndi kukwanda pasi. Posilizila Yosefe na Rakele ana bwela na kugwanda. ⁸ Esau anakamba, " Utanthauza ciani pa banthu wonse aba bambili nakumana nao?" Yakobo anakamba, " Kuti nipeze mwayi pameso pa bwana wanga." ⁹ Esau anakamba, " Nili nazo zokwanila, mbale wanga. Zisungele zonse zamene ulinazo." ¹⁰ Yakobo anakamba, " Yai, napapata, Ngati napeza mwayi pa menso panu, nipempa kuti mulandile mpaso iyi yofumila m'manja yanga. 200 nadi naona pa maso pano, cili nga nikuona pa maso pa Mulungu, ndipo mwani landila ine. ¹¹ Napapata landilani mpaso yanga yamene nakubweleselani ine, cifukwa Mulungu wacita naine mwa cisomo, ndipo ndili nazo zokwanila," Pamene Yakobo anamupapatila, Esau analandila mpaso ija. ¹² Ndipo Esau anakamba, "Tiyeni tiyambepo kuyenda, ine nizakhala pa songolo panu." ¹³ Yakobo anamu uza iye, " Mbuye wanga zibani ici kuti bana nibang'ono, ndi mbelele ndi ng'ombe zinyonsha tubana. Ngati tizayenda mwa mpavu cukanga siku imodzi cabe zibeto zizafa. ¹⁴ Napapata lekani bwana ayende patsongolo pa kapolo wanu. Nizayenda pangono pang'ono, ngani mwazibeto zamene zili ku songolo, ndi monga bana, kufikila tifike kwa bwana wanga ku Seiri." ¹⁵ Esau anakamba, " Lekani nikusiyileni amuna banga amene bali na ine" Koma Yakobo anayankha, " Ciani mzacitila izo? Lekani nipeze mwayi pamanso ya bwana wanga." ¹⁶ Ndipo Esau pa siku ija anayambapo ulendo wake kupita ku Seiri. ¹⁷ Yakobo anayenda ku sokoti, kukazimangila iye mwine nyumba na makolo ya zibeto zake. Ndipo zina la malo ndi Sokoti. ¹⁸ Pamene Yakobo anacoka kufumila ku padamu Aramu, anafika bwino ku mzinda wa Shekemu, malo yopezeka mu Kenani anaphumulila pafupi ndi mzinda. ¹⁹ Ndipo anagula malo pamene anamangila Hema kucokela ku mwana wa Hamo, tate wa Shekemu, ndi mutengo wa Hundriredi ziduswa za siliva. ²⁰ Kuja anamanga guwa ndikuipatsa zina kuti Eli Elone Isilayeli.

Chapter 34

¹ Manje Dina mwana wa Leya wamene ana bala kuli Yakobo anayenda kukumana akazi aci cepele bamu malo. ² shekemu mwana wa hamori mu Hiviti, mwana mwamuna obadwa ku mfumu wamu malo, ana muona. Ana mutenga ndi kugona naye ndi kumu citisa manyazi. ³ Ana tenga mutima na Dina, mwana wa Yakobo. Ana mukonda mukazi waci cepele ndi kukamba naye mo ndenka. ⁴ Shekemu ana kamba na atate bake Hamori kuka kamba kuti, "Tengani mukazi mungono uyu ankale mukazi wanga." ⁵ Manje Yakobo ana nvela kuti, ana muonga Dina mwana wake. Bana bake ba muna banali na zibeto zake mu sanga, ndipo Yakobo analigwila mutendele panku bana bwela. ⁶ Hamori tate wa Shekemu ana yenda kuli Yakobo ku kamba naye. ⁷ Bana bamuna ba Yakobo bana bwela ku coka kusanga pamene bana nvela za ici. Bamuna bana kwiyisida bana kalipa maningi cifukwa Israeli ananvesewa manyazi posona na mwana wa Yakoba mukazi, chintu moonga ici sicalina kufunika kuchitika. ⁸ Hamori ana kamba na beve, kuti, "Mwana wanga Shekemu akonda mwana wamunu mukazi napapata mupaseni ankale mukazi wake." ⁹ Tikwatilane, tipaseni bana banu bakazi, ndipo tengani bana bathu bakazi kwa imwe. ¹⁰ Muzankala naise ndi pamalo pazankala po seguka kuli imwe kunkala ndi ku gulisa ndi ku gula ka tundu." ¹¹ Shekemu ana kamba kuli batate bake ndi abale bake. "Lekani ni peze mwai pa menso panu ndi vamene vili vonse muza kamba niza kupasani. ¹² Nifunseni pali vintu vikulu monga lobola na mphaso mwamene munga funile, ndipo niza kupasani vilivonse vamene muza ni uza, koma nipaseni mukazi wa ci cepele ankale mukazi wanga." ¹³ Bana bamuna ba Yakobo bana yanka shekemu na Hamori tate wake mo nama, chifukwa Shekemu anaonga Dina mulongo wabo. ¹⁴ Bana kamba kuli beve, "Sitinga cite ici, ku pasa mulongo watu kuli aliyense osa dolidwa, ndipo ice cingankale ca ci soni kuli ise. ¹⁵ Pali ici cabe ndiye pamene tizanelana na imwe: Ngati uzankala odolidwa moonga ise, ngati mwanuna onse paimwe nadolidwa. ¹⁶ Ndiposo tiza pasa bana batu bakazi kuliimwe, ndiponso tiza teza tenga bana banu bakazi kwa ise, ndipo tizankala pamozi nakunkala bantu ba mozi. ¹⁷ Koma ngati simuti nvela ndi kudolidwa, ndiponso tiza tenga mu mulongo watu ndi kuyenda." ¹⁸ Mau yabo yana muko ndwelesa Hamori ndi mwana wake Shekemu. ¹⁹ Uyu munyamata sana cedwe kucita vamene bana kamba, cifukwa anali okodwela mu mwana mukazi wa Yakobo, na chifukwa chakuti enzeli munthu wo lemekezeka maningi munyumba yatate bake yonse. ²⁰ Hamori na Shekemu mwana wake mwamuna bana yenda pongenela mu mzinda wabo naku kamba naba banthu bamzinda, kuti, ²¹ "Aba bantu bana mtendele naise, balekeni bankwe mu malo na kugulisilamo, zoonadi, aya malo niya kulu yobkwanila. Lekani titenge bana babo ba kazi bankale bakazi bathu, naku ba pase bana batu bakazi. ²² Pali ici cabe banthu aba ndiye pamene aba banthu baza vomela ku nkala naise na kunkala banthu ba mozi, ngati bamuna bonse pakati paise nebo dolidwa, mwamene balili odolidwa. ²³ Kansi vobeta vabo na katundu yabo nyama zao zonse sivilizankala watu? Ndipo tivomelezane, nabo na kunkala pakati patu." ²⁴ Banthu bonse bamuzinda bana nvelela Hamori na Shekemu, mwana wake mwa muna. Bamuna bonse bana dolidwa. ²⁵ Pasiku ya ci tatu, pamene banali kunvela ku baba, pabana babili ba Yakobo (Simeon ndi Levi abale ba Dina), aliyense anatenga lupanga naku menya mzinda wamene unali ukutila nacicitezo cake, naku paya bamuna bonse. ²⁶ Bana paya Hamori na mwana wake mwamuna Shekemu kusebenzesa lupanga. Bana tenga Dina ku coka ku nyumba kwa Shekemu nakuyenda. ²⁷ Bana ba Yakobo bamuna benangu bana bwela kuma tupi yao kufa naku bela mzinda, chifukwa aba banthu bana ononga mulongosi wabo. ²⁸ Bana tenga vobeta vabo, ngombe zabo, aburu na vonse vamu mzinda na va minda yoba zunguluka. ²⁹ Cuma cabo conse. Bana bao bonse na ba kazi babo bana guliwa. Bana tengela pamozi na vonse vamu manyumba. ³⁰ Yakobo ana kamba kuli Simeon na Levi "Musaletе so vuta pali ine, kuni lengesa ku nunka kuli bonkala mu malo yano, akenani na Aperiziti ndine ocepe muku penda. Ngati ba zakumana bonse pamozi naku nicita cipongwe, ndipo nizaonengeka ine naba munyumba yanga." ³¹ Koma Simeon na Levi ana kamba, "Kodi Shekemu Enzekufuna mulongosi wanthu moonga ni hule?"

Chapter 35

¹ Mulungu ana uza Yakobo, "nyamuka, yenda mpaka kufikila ku Bethel, Ndipo ankale kwamene kuja. Manga guwa kwamene kusa ya mulungu, wamene ana oneka kuli iwe pamene anataba kuli Esau mubali wako. ² Ndipo Yakobo anauza ba munyumba yake na bonse bamene anali nabo, "ikani kutali tu milungu twa kunja twamene tuli naimwe, ziyeeleseni mweka, ndipo chinjani vovala vanu. ³ Ndipo tiyeni tiyambeko na kuyenda mpaka kufikila ku Bethel niza manga guwa kuja ya Mulungu, wamene ananiyanka mu musiku yo tangwanika, na ku nkala naine kuli konse kwamene nayenda." ⁴ Mwaicho banamupasa Yakobo tonse mulungu twa boza twamene tunali mu manja mwao, na masikiyo ya mene yanali ku matu yao. Yakobo anayafwikila mangansi mwa mutengo wathundu unali pafupi na she chem. ⁵ Pamene banali kuyanda, Mulungu anapanga manta kugwela pa mizi zamene zanali kuba Sibaha bakonke bana ba Yakobo. ⁶ Mwaicho Yakobo anafaka ku Luz (amene inali Bethel), yamene inali kumalo yaku Kanaani, eye na bonse bantu bamene banali naye. ⁷ Anamanga guwa kuja na kupasa Mulungu anazi onesa kuli eve pamene anali kutaba ku chokela kuli mu bale wake. ⁸ Deborah, wachinto wa Rabekal, anafa. Anashikiiwa ku Bethel pansu pa mutengo wathundu, mwaicho bana itana malo yaja Allon Bakuthi. ⁹ Pamene Yakobo anabwela kuchoka ku Paddan Aran, Mulungu anaonekela kuli eve naku mudalisa. ¹⁰ Mulungu anakamba kuli eve, "Zina yako si Iza itaniwa Yakobo. zina yako izanikala Iseali." waicho Mulungu anamuitana zina yake Isreali. ¹¹ Mulungu anakamba kuli eve, "ndiwe Mulungu wampamvu zonse. Kaba laneni na kupaka. Ziko na magulu ya maiko yazachoka kuli imwe, pa bana banu. ¹² Malo yamene nina pasa iwe ku bana bo badwa mumbuyo mwako. niza bapasa malo." ¹³ Mulungu anachokako ku malo kwamene nanakamba na naye. ¹⁴ Yakobo anaika mwala ukulu pamalo pamene Mulungu anali ku kamba naye. Pila ya mwala. Anafilapo chakumwa kunkala ngati nsembe na mafuta. ¹⁵ Yakobo anaitana malo yamene Mulungu analikukamba naye, bethel. ¹⁶ Banali pa ulendo kuchokela ku Bethel, Rakel vumo inauka. ¹⁷ Pamene vumo inauka mo vuta, omubalisa anamu uva, "osayopa, apa manja uzankala na mwana mwamuna winangu. ¹⁸ Pamene anali kufa, anaku pema ko silizila anapasa zina mwana wake Ben-oni, koma atate bake banamuitana Benjamin. ¹⁹ Rakel anafa ndipo banamu shika munjila yo yenda ku efrata (ndiye Bethlehem). ²⁰ Yakobo anaikapo mwala pa manda pake ni chozibilako pa manda pa Rakel mpaka lelo. ²¹ Isreali anayenda na kufika hema yake pasogolo pa yanganila vibeto vake. ²² Akali kunkala kumalo kuja, Reubeni anagona na Bilhah nukazi wa atate bake waku mbali, na Isreali ananvela pali iyi nkani. ²³ manji Yakobo anali na bana bamuna 12. Bana bake kuli Leya banali Reubeni, mwana wkae oyamba, ana Simeoni, Levi, Yudah, Isacha, na Zebulani. ²⁴ Bana bake kuli Rakel banali Yosefe na Benjamin. ²⁵ Bana bake kuli Bilhah wa nchito wachikazi banali Dani na Naphatali. ²⁶ Bana ba Zelipa, wachoto wa Leya mukazi, banali Gad, na Asher. Bonse aba banali bana ba Yakobo bamene anabala ku Paddan Aram. ²⁷ Yakobo anayenda kuli Isaki atate bake, ku Mamre mu Kinah Arba (chimozimozi Hebron) kwamene Abrahamu na Isaki banali ku nkala. ²⁸ Isaki anankala zaka 108. ²⁹ Isaki abapema ka kosilizila nakufa, ndipo anatengewa ku makolo yake, nkalamba ya masiku yambili. Esau na Yakobo, mwana wake mwamuna, banamushika.

Chapter 36

¹ Aba ndiye ba nali mibadwo ba Esau (ozibika futi ati Edomu). ² Esau anatenga bakazi bake ku chokela kuma kanani. Aba ndiye bakazi bake: Adahi mwana mukazi wa Eloni waku Hittite; Oholibamah mwana mukazi wa Ana, muzukulu zw Zibioni waku Hivitte; ³ na Basemathi, mwana mukazi wa Ishmaeli, mulongosi wa Nebaiioth. ⁴ Ada anabala Elifazi kuli Esau, na Basemati anabala Ruweli. ⁵ Oholibama anabala Jeushi, Jalami, na Kora. Aba ndiye banali bana bamuna ba Esau banabadwa kuli eve mu malo ya Kenani. ⁶ Adahi ana bala Eliphaz kuli Esau, kuchoka apo Basemathi ana bala Reueli. oholibamah ana bala Jeushi, Jalam, na Korah. Aba ndiye ba nali bana bamuna ba Esau bana badwila ku malo ya Kanani. Esau anatenga bakazi bake, bana bake bamuna, bana bake bakazi na bonse bapa nyumba yake, na vobeta vake - navi nyama vake vonse, na vintu vake vonse, vamene anafaka pamozi ku malo ya kanani, naku chokako ku malo kuli mubale wake Yakobo. ⁷ Ana chita chifukwa vinthu vabo vina paka kuti sibanga nkale pamozi. malo yamene bana nkhalapo siyi nakwanile kuba thandizila chifukwa chavobeta. ⁸ Kuchoka apo Esau, Esau ozibakanso Edomu. ana nkhalala ku ziko ya seir. ⁹ Aba ndiye ba nali midadwo ba Esau, makolo bama Edomite ku ziko ya seir. ¹⁰ Aya ndiye yanali mazina ya bana ba muna ba Esau: Eliphazi mwana mwamuna wa Adahi, mukazi wa Esau; Reueli mwana mwamuna wa Basemathi, mukazi wa Esau. ¹¹ Bana bamuna ba Eliphazi benze Temani. Oma, Zifo, Gatami, na Kenazi. ¹² Timna, mpali ya Eliphazi, mwana mwamuna wa Esau, anabala Amaleki. Aba ndiye banali ba Zukulu ba Ada mukazi wa Esau. ¹³ Aba ndiye banali bana bamuna ba Reueli: Nahati, Zera, Shama, Mizza. Aba ndiye banali bazukulu Basemathi, mukazi wa Esau. ¹⁴ Aba ndiye banali bana bamuna ba Oholibama, mukazi wa Esau, enzeli mwana mukazi wa Ana na muzukulu mukazi za ZibiyoniAnamu balila Esau Jeushi, Jalami, na Kora. ¹⁵ Uyu ndiye mutundu pali mibawo wa Esau: mibadwo wa Eliphazi, mwana oyamba wa Esau: Temani, Oma, Zifo, Kenazi, ¹⁶ Kora, Gatami, na Amaleki. Ndiye yenzeli mutundu yamu mibabdwwo ya Eliphaz ya Edom, Banali bazukulu ba Ada. ¹⁷ Uyu ndiye unali mutundu wa Reueli, mwana mwamuna wa Esau: Nahati, Zera, Shama, Mizza, Uyu ndiye unali mutundu obadwila klui Reueli ku malo ya Edomu. ndiye banali bazukulu ba Basemati, mukazi wa Esau. ¹⁸ Uyu ndiye unali mutundu wa Oholibama: mukazi wa Esau: Jeush, Jalam, Kora. Uyu ndiye mutundu wa mibabdwwo wa mukazi wa Esau Oholibama, mwana mukazi wa Ana. ¹⁹ Aba ndiye banali bana bamuna ba Esau (ndiye futi Edomu), aba ndiye banali ma mfumu. ²⁰ Aba ndiye banali bana Seya waku Horiti, bonkhala pa malo: Lotani, Shobali, Zibiyoni, Ana, ²¹ Dishoni, Eze, na Dishani. Uyu ndiye mutundu wama Horiti. bamene ba nkhalala ku Eya pa malo ya Edomu. ²² Bana Lotani benzeHori na Hemani, na Timna mulongosi wa Lotani. ²³ Bana bamuna ba Shobali: Alvan, Manahati, Eballi, Shefo, na Onamu. ²⁴ Aba ndiye banali bana bamuna ba Zibiyon: Aiah na Ana. Uyu ndiye Ana anapeza kamugodi ka manzi youkupya muchululu pamene enze kudyesa ma donke ya Zibiyoni tate wake. ²⁵ Aba ndiye banali bamu ba Ana: Dishoni na Oholibama, mwana mukazi wa Ana. ²⁶ Aba ndiye banali bana bamuna ba Dishoni: Hemdani, Eshabani, Ithran na Kerani. ²⁷ Aba ndiye banali bana bamuna ba Eze: Bilhan, ZAavani, na Akani. ²⁸ Aba ndiye banali bana bamuna ba Disheni: Uz na Arani. ²⁹ Uyu ndiye unali mitundu wama Horites: Lotani, SHobali, Zibiyoni, na Ana, ³⁰ Dishoni, Ezeri, Dihani: izi ndiye zinali mitundu zama Horites, kulingana na mitundu wapa malo ya Seya. ³¹ Izi ndiye mfumu zinal ku lamulila pa malo ya Edomu pamene ili yonse ikalibe ku lamulilapa pali bana bamuna ba Isireli: ³² Belai mwana mwamuna wa Bowa, ana lamula Edom, na zina ya muzinda yenzeli Dinhabah. ³³ Pamene Belai anafa, ndiye Jobabi mwana mwamuna wa Zera waku Bozrah, ana lamulila pa malo pake. ³⁴ Pamene Jobabi anafa, Hushami enze waku malo kwa ma temanites, ana lamulila pa malo pake. ³⁵ Pamene Hushami anafa, Hadadi mwana mwamuna wa Bedadi wamene ana konjesa ma midiantes mu malo ya Moabi, ana lamulila pa malo yake . zina yamu muzunda inali Aviti. ³⁶ Pamene Hadadi anafa, ndiye pamene Samlahi waku Masrekah ana lamulila pa malo yake. ³⁷ Pamene Samlahi anafa, ndiye Shauli waku Rehoboth ku kamumana ana lamulila pa malo yake. ³⁸ pamene Samlahi anafa,ndiye pamene Baal-Hanani mwana mwamuna wa Akbor, ndiye ana lamulila pa malo yake. ³⁹ pamene Baal-Hanani mwana mwamuna wa Akbor, anafa, ndiye pamene Hadar ana lamulila pa malo yake. Zina ya muzinda yake yenzeli Pau. Zina yamu kazi wake inali Mehetabeli mwana mukazi wa Me Zahab. ⁴⁰ Aya ndiye yanali mazina yaba sogoleli ku chokela kuli mibabdwwo ya ESau, kulingana na mitundu na chigau chao. am Zina yabo: Timna, Alvah. Jethehi, ⁴¹ Oholibama, Elahi, Pinon, ⁴² Kenaz, Temani, Mibzar, ⁴³ Magdiel, na Irami. Aba ndiye banali ba sogoleli ba Edomu lulingana nama nkaliidwe mu malo yamene bana tenga. ndiye enze Esau, tate wama Edomites.

Chapter 37

¹ Yakobo anankala mu malo ya Kanani, mwamene anankalamo batate bake. ² Ivi ndiye vinachitika pa umoyo wa Yakobo, Yosefe, wamene anali munyamata mufana wa zaka seventini, anali kulonda vinyama nazibale bake. Anali na bana ba Bila na bana ba Zelipa, bakazi ba batate bake. Yosefe anali kubaletela lipoti yoyipa kuli tate wawo. ³ Koma manje Isilayeli anakonda Yosefe manigni kupambana na bana bake bamuna bonse chifukwa ndiye mwana anabadwa Yakobo atakalamba pa bana bamuna bonse. Anamupangila chovala chabwino maningi. ⁴ Babale bake banaona kuti batate babo amukonda maningi kuchila na pa bana bonse. Anamuzonda andipo sanalikukamba naye bwino mwa chifundo. ⁵ Yosefe analota maloto, naku uza babale bake viloto vamene ivi. Banamuzondelako maningi. ⁶ Anakamba kuli benve kuti, Napapata nvelani maloto yanga yamene na lota. ⁷ Onani, tinali kumanga mitolo ya vamumunda ndipo onani, mutlolwanga unayamuka nakuyimilila kuyanga kumwamba, ndipo onani, mitolo yanu inabwela mumbali zonse nakubelamila mutolo yanga. ⁸ Babululu bake banakamba kuli enve kuti, "Zo'ona uzatilamilila ise? uzatisogolela zo'ona ise? Banamuzondelako enve chifukwa chamaloto yake na mau. ⁹ Analota maloto yenangu naku uzako babale bake. Anakamba kuti, "Onani, nenze nalota loto inangu: Zuba na mwezi na nyenyezi zili leveni zinali kugwadila ine." ¹⁰ Anayenda kukamba maloto kuli batate bake chimozi mozi mwamene anauzila babale bake, ndipo batate bake anamukalipila. Anakamba kuli enve kuti, "namaloto yamu tundu bwanji aya yamene walota? ushe vizakachitika zo'ona kuti bamai bako naine naba bale bako tizabwela naku kugwadila pansi kuli iwe? ¹¹ Abale bake banamuchitila jelasi, koma batate bake banasungila iyi nkani mumutima mwao. ¹² Ba bale bake banayenda kukadyesela vinyama va batate babo ku Shekemu. ¹³ Isilayeli anakamba kuli Yosefe kuti, "kodi azibale bako sibanyende kudyesa vinyama ku Shekemu? Bwela ndipo nizakutuma kuli benve." Yosefe anakamba kuli batate bake, "Ndine okonzeka." ¹⁴ Anakamba kuli enve kuti, "Yenda manje, ukaone ngati vibayendela bwino benve navi nyama, ndipo uniletele mau." Ndipo Yakobo anamutuma kuchokela ku vale ya Hebroni ndipo Yosefe anayenda ku Shekemu. ¹⁵ Muntu winangu anamupeza Yosefe ali kuyenda musanga. Mwamuna uja anamufunsa "Usakila chani?" ¹⁶ Yosefe anayanka kuti nisakila azibale anga, niuzeni, nisakila zaiblae anga, miuzeni napapata, kwamene balikudyesela vinyama. ¹⁷ Mwamuna uja anati, "Banachokako kuno, ndaba na banvela bakamba kuti, tiyeni ku Dotani." Yosefe anaba konkamo ba bale bake bapeza ku Dotani. ¹⁸ Banaona bakali kutali, ndipo bakalibe kufika pafupi nabenze, bana pangana mwachiwembu kuti amupaye. ¹⁹ Ba bale bake banakambisana kuti, "Onani, Uyu wamaloto wabwera pafupi. ²⁰ Bwelani manje apa, chifukwa chake, tiyeni timupaye timuponye mu umozi mu mugodi ilikuno. Tizakamba kuti, 'Chinyama chamusanga chinamudya. ' Tizaona vamene maloto yake yazasanduka." ²¹ Rubeni anamvela iyi nkani nakumupulumusa mumanja mwao. Anakamba kuti, Tisamu paye." ²² Rubeni anakamba kuli benve kuti, "Osakesa magari muponyeni mumu godi uyu uli kuno kusanga, koma asamu kumyako kwanja, "pofuna kuti angamupulumuse kumuchosa mumanja mwao nakuyenda kumupeleka kumubweza kuli batate bake. ²³ Chinachitika kuti pamene Yosefe anafika pali bazibale bake, banamu vula chovala chake chokongola. ²⁴ Banamutenga nakumuponya mumugodi munalibe chintu, ndipo munalibe manzi mukati. ²⁵ Bana nkala pansi kuti badye buledi. Bananyamula menso yabo nakuona, ndipo, onani, kunali kalavani yama Ishamealiti inali kubwela kuchokela ku Giliyadi, nama kamelo yabo yonyamula masipayisi na balami na mure. Banali paulendo bopeleka iyi katundu ku Iguputo. ²⁶ Yuda anakamba kuti kuli ba bale bake, "Pali pindu yabwanji ngati tizamupaya mubale watu nakubisa magari yake? ²⁷ Bwelani, ndipo tiyeni timugulise kuli ma Ishiamyeliti ndipo tisakumyepo manja yatu pali enve. Pakuti nimubale watu, magari yatu, " Ba bale bake banamunvelela iyi. ²⁸ Mamechanti baku Midiyani banapitila pafupi. Ba bale bake banamudonsa Yosefe nakumunyamula kumuchosa mumugodi. Banamugulisa Yosefe kuli ma Ishimayeleti pa mutengo wa twenti ndalama za siliva. ndipo ma Ishimayeleti anamunyamula Yosefe kuyenda naye ku Iguputo. ²⁹ Rubeni anabwelelapo pamugodi, ndipo onani, Yosefe analimo mumugoidi. ³⁰ Iye anang'amba vovala vake. Anabwelela kuli bazibale bake nakukamba kuti munyamata salimo! ndipo ine nizayenda kuti?" ³¹ Banapaya mbuzi naku tenga malaya ya Yosefe nakuya sunsika mu magari. ³² Pamene banaleta chija chovala kuli batate babo nakukamba kuti, "Tapeza ichi. Tapapata chiyanganeni ngati ni chovala chamwana wanu kapena olo sichamene." ³³ Yakobo anachiziba nakukamba kuti, "Nichoavala cha mwana wanga mwamuna. Chinyama chamusanga chamudya. Yosefe akazuliwa zo'ona mumapisi na chinyama." ³⁴ Yakobo anang'amba vovala vake naku vala ³⁵ chovala chamsaka mumusana. Analila mwana wake mwamuna masiku yambili. ³⁵ Bonse bana bake bamuna na bakazi bananyamuka kumu tandiza kulila momupepesa, koma anakana kumuchita kamfoti. Anakamba kuti, "Zo'ona nizayenda ku Shilo nikalikulila mwana wanga." Batate nake banalila mokuwa kamba ka enve. Ma Midiyanaite yanamugulisa mu Iguputo kuli Potifa mu ofisala wa Farao, mukulu wama bodigadi.

Chapter 38

¹ Inabwela ntawi pomwe Yuda anasiya abale bake nonkhala kuli omwe anali na zina la Hira. ² Anapeza kuja mwana mukazi wa mwamuna waku Kenaani anali na zina la Shuwa. Anamutenga ndipo anamungela. ³ Anankhala na mimba na bala mwana mwamuna. Anamupasa zina la Eri. ⁴ Anankhala na mimba nafuti nomabala mwana mwamuna. Anamupasa zina la Onani. ⁵ Anankhala na mwana mwamuna nafuti nomupasa zina Sela. Kunali ku Kezib kwe anamubalila. ⁶ Yuda anapezela Eri mwana wake woyambilila, mukazi wo kwatila zina lake anali Tama. Eri, mwana wa ⁷ Yuda wo yamba, analiuchita zo chimwa pa menso ya Yehova. Yehova anamupaya. ⁸ Yuda anati kuli Onani, "ngenela mukazi wa Abbale bako. Chita nchito yamulamu mwamuna kuli eve, kuti ukulise mwana wamu abale bako." ⁹ Onani anaziba kuti bana zibaza nkhalake. Lyonse akangena kumukazi wamu bale wake, anatila pansu mpavu vachimuna kuti anankhale na mwana wa abale ake. ¹⁰ Ve anachita venze vochimwisa pa menso ya Yehova, Yehova anamupaya na eve. ¹¹ Yuda anati kuli Tama, muungozi wake, "Upitise kunkhala wofesdwa munyumba yabatate bako kafika sela, mwana wanga, akakule." chifukwa anayopa, "Kuti angafe nayeve, monga abale bake." Tama ayenda kunkhala munyumba yabatate bake. ¹² Patapita ntawi itali, mwana mukazi wa Shua, mukazi wa Yuda, anafa. Yuda bana mutontoza ndipo anayenda kuli bo embela mbelele zake ku Tina, eve namukaze Hira waku Adulamayiti. ¹³ Tama bana muwuzi, "wona, ba pongozi bako bamuna bayenda ku Tina kuyembela mbelele zake." ¹⁴ Anachosa zovala zamukazi wafedwa ndipo anazivwinikila na nyula nozimanga. anakhala pongenela mumalo ya Enami, inali pambali pa njila yaku Tina. chifukwa anawona kuti Sela akula koma sibanamukwatilise kuli eve. ¹⁵ Pamene Yuda anamuwona anaganiza monga nimukazi wachiwele wele chifukwa enze anabisa nkope yake. ¹⁶ Anyenda kuli eve ndipo anti, "Bwela, leka naiwe chifukwa sana zibe kuti nimupongozi wake mukazi ndipo mukazi anakamba kuti, "Uzani pasa chani ukagona naine?" ¹⁷ Mwamuna anakamba kuti, "Niza kutumila kambuzi kang'ono kuchoka kuzobeta." mukazi anakamba kuti, "uzampasa lowezo kufikila ukatume?" ¹⁸ Mwamuna anakamba kuti, "Nilonjezo bwanji yeningakupase? mukazi anayanka, "chidindo na ntambo yako na ndondo ili mumanja yako." Anamupasa no yenda kuli eve, ndipo anankhala na mimba yake. ¹⁹ Mukazi anayima noyenda njila yake. Anachosa nyula yake no vala zovala za wofedwa. ²⁰ Yuda anatumiza ka mbuzi kang'ono kupitiula mumunzake waku Adulamayiti kuyi angetenge lonjezo lake kuchokela mumanja yamukazi, kuno sanamupeze. ²¹ Waku adulamayiti anafunsa ba muna ba pa malo, "alikuti mukazi wachiwelwewe enze pa mbali pa njila ya Enami?" Banakamba kuti, "kunalibe mukazi wachiwelwewe pano." ²² Anabwele kuli Yuda anakamba kuti, "Sinamupeze. Nabamuna ba pamalo banakamba kuti, 'kuliba mukazi wechiwelewele pano.'" ²³ Yuda anakamba kuti, mutekeni usunge vintu, kuti tisaletelwe nsoni, chifukwa, nonatuma ka mbuzi kang'ono koma sanamupeze." ²⁴ Pekunapita myezi itatu uda banamuza kuti, "Tama mupongozi wako mukazi achita zawewelele, ndipo anankhala mimba." Yuda anakamba kuti, "Muleteni kuno timushoke." ²⁵ Pabanamuleta panja, anatuma utenga kuli bapongozi bake, "Ninamimba ya mwamuna alina vintu ivi." Mukazi anakamba kuti, "Sakilani mwine wa ivi, chofundo na ntambo na ndondo." ²⁶ Yuda anaviziba no kamba kuti, "Ni wolungama kuchila ine. chifukwa sinina mukwatolise ku mwana wanga, Sela." ²⁷ Pamene inafika ntawi yonkala na mwana, Onani, bampundu banli mumala. ²⁸ Inafika pamene eze ku bala umozi anachosa kwanja panja, ndipo wabalisa anatenga ka ntambo ka redo no kamanga pa kwanja nokamba kuti, "Uyu ayambilila kuchoka." ²⁹ Koma pamene ana bweza kwanja, ndipo, Onani, bale wake anayambilila kuchoka. Wabalisa anakamba kuti, "Mwewachokela!" Ndipo bana mwitana kuti Perezi. ³⁰ Bale wake anachika, anali naka ntambo ka redi pa kwanja, ndipo bana mwitana kuti Zera.

Chapter 39

¹ Yosefe ana letewa ku Egipito. Potifa, mu sogoleli wa Farao wamene anali muklu wama malonde waku Egipito, anamu gula kuli ma Ishmaelites, wamene anamaleta kuja. ² Yehova anali na Yosefa ndipo ana nkala olemela kwambili. Ana nkala mu njumba ya bwana wake waku Egipito. ³ Abwana bake bana ona kuti Yehova anali na Yosefe na zonse zamene anali kuchita yehova ana chulukisa. ⁴ Yosefe anapeza mwai. Anamu sebezela Potifa. Potifa anapanga Yosefe bwana wapa nyumba yake, navonse vintu vake, anavi ika mu manja mwake. ⁵ Zina chitika kuti choka pamene ana nkhalala musogoleli wapa nyumba na vonse vintu, Yehova anadalisa nyumaba yawaku Egipito chifukwa cha yosefa. Daliso ya Yehova inali na vonse vintu va Potifa vamu nyumba namu munda. ⁶ Potifa ana ika vonse vintu vake mumanja ya Yosefa. Sanali kufunika ku ganiza pali chili chonse koma chabe chokunya chamene eze kudya. Ndipo Yosefa anali wa bwino nakuoneka bwino. ⁷ Zina chitika ku choka apa kuti mukazi wa bwana wake anamu kumbwila Yosefe no kamba, "Gona na ine." ⁸ Koma anakana ku gona naba kazi ba abwana bake, "Ona, bwan wanga sama ikako nzelu ku vonse nichita mu nyumba yabo, anani ika ku langanila vonse vintu vabo." ⁹ Kulibe mwamukulu mu nyumba muna pali ine sana bisa kantu kuli ine koma iwe, chifukwa ndiwe mukazi wake. Ninga chite bwanji zo ipa izi naku chimwila Mulungu?" ¹⁰ Anakamba na Yosefa siku na siku, koma anakana ku ngona nabo olo ku nkala naye. ¹¹ Zina chitika kuti siku imozi anayenda ku sebenza ku nyumba. Amuna bonse sibana liko mu nyumba. ¹² Anamu gwila pa chovela naku kamba, "Gona na ine." Anasiya chovala mu manje yake, kutaba, kuyenda panja. ¹³ Ina bwela kuti, pamene anaona kuti psaya chovala mu manja naku tabila panja, ¹⁴ ana itana amuna ku nyumba naku bauza kuti, "Ona, Potifa ati letela muntu wachi Hebeli kuti sobelesa. Ezeli abwela kuti agone na ine ndipo napunda." ¹⁵ Zinaditika pamene napunda, ataba kusiya chovala naine, nakuyenda panja." ¹⁶ Ana ika chovala chake pafupi na eve mpaka ba bwana bake ba bwela ku nyumba. ¹⁷ Anamu londolela izi, "Mu Hebeli wa nchito wamene unaleta kuli ise, eze abwela kuni sobelesa." ¹⁸ Zabwela za chitika kuti pamene napunda, ataba kusiya chovala chake naine, atabila panja." ¹⁹ China chitika, pamene abwana ana vela ku londolola kwaba kazi abo, "Ichi ndiye chamene wa nchito wako achita kuli ine," Ana kalipa kwambili. ²⁰ Abwana ba Yosefa banamutenga naku ika mu ndende, mu malo mwamene akaidi ba mfumu banali. Ezeli mu ndende. ²¹ Koma Yehova anali na Yosefa nakumu onese ku kulupilika kwachi pangano. Anamu pasa mwai mu menso yao olonda ndende. ²² Olonda ndende ana pasa mu manja mwa Yosefe bonse akaidi banali u ndende. Vilivonse vamene bana chita kuja, Yosefe anali oyanganila. ²³ Olonda ndende sanade nkawa pali chili chonse chinali mu manja yake, chifukwa Yehova anali na eve. Zili zonse zamene ana chita, Yehova ana chulukusa.

Chapter 40

¹ Zinabwela pambuyo patapita ivi vintu, wopelekela chakumwa kwa mfumu ya ku Igupto ndi wopanga buledi anakalipisa bwana wawo, mfumu ya ku Igupto. ² Farao anakalipila banchito bake bakulu bakulu babili, mukulu opeleka chakumwa na mukulu bopanga buledi. ³ Anabaika mu jele mu nyumba ya malonda mukulu, mu jele mwamene Yosefe analili. ⁴ Mukulu wa bamalonda anabapeleka mumanja uya Yosefe, ndipo iye anabasamalila. Bana nkhalu mu jele kwa kantawi. ⁵ Bonse babili bana lotta chiloto, wopasa chakumwa na opanga bulendi ya mfumu ya ku Igupto pamene banali mu jele. Aliyense anali na chiloto usiku umozi, ndipo chiloto chili chonse chinali ndi chivumbuluso. ⁶ Yosefe anabwela kuseni mukubaona. Onani banali osakodwela. ⁷ Anafunsa bakulu bakulu ba Farso bamene banali naye mu jele mu nyumba ya bwana wawo, nati nanga nichani muoneka osakondwela lelo? ⁸ Iwo bana muyanka, bonse talota chiloto ndipo kulibe aliyense angamasulile. " Yosefe anabauza, " Kodi kumasulila sikwa Mulungu niuzeni, napapapta." ⁹ Mukulu opeleka chakumwa anamu uza chiloto chake Yosefe. Anamu uza kuti, onani, mutengo unali pasongolo panga. ¹⁰ Mumutengo munali ntambi zitatu. Pamene unapulika, maluba anachoka ndipo unabala mpesa zakupya. ¹¹ Chiko cha Farao chinali mumanja mwanga. Ninatenga mpesa nakuzi fyanila mu chiko cha Farao, ndipo ninaika chiko mumanja mwa Farao." ¹² Yosefe anati kwa iye, iyi ndiye tantauzo lake. Ntambi zitatu ni masiku atatu. ¹³ Mu masiku yatatu Farao azakuchosa mu jele nakukubweza pa chito yako uzaika chiko mumanja mwa Farao, monga mwamene unalili opeleka chakumwa. ¹⁴ Koma ukaniganizileko zikayenda bwino naiwe. Ukamu uze Farao pali ine kuti akani choseko muno mu jele. ¹⁵ Popeza ine ninali monga ogwiliwa kuchokela ku ziko la Ahebri, ngankhale kuno, sininalakwe kali konse kuti ni pezeke mu jele muno." ¹⁶ Pamene mukulu opanga bulendi anaona kuti kuvumbulusa kunali bwino, anati kwa Yosefe, " Naine nenze na chiloto ndipo, onani mabasiketi yatatu ya buledi yanali pa mutu panga. ¹⁷ Mu basiketi ya pamwamba munali zosiyana siyana za kudya za Farao, koma tunyomi tunadya mu basiketi inali pa mutu panga." ¹⁸ Yosefe ana yanka nati, " Iyi ndiyo tantauzo. Mabasiketi yatatu ni masiku atatu. ¹⁹ Mu masiku yatatu Farao azakuchosa mu jele ndipo azakupachika pa mutengo. Ndipo tunyoni tuzadya tupi yako. ²⁰ Kunabwela kuti pasiku la chitatu, linali siku lakukumbukila kubadwa kwa Farao. Anapanga madyelelo yabanchito bake bonse. Kumwa na mukulu wopanga buledi, kuli ba nchito bake. ²¹ Ana mubweza panchito yake mukulu wopeleka chakumwa ndipo anaikanso chiko mumanja mwa Farao. ²² Koma anapachika mukulu wa opanga buledi, monga mwamene Yosefe anavumbulusila kwa iwo. ²³ Koma mukulu wa opeleka chakumwa uja sanamukumbukile Yosefe, ndipo anamuibala.

Chapter 41

¹ Pamene panapita zaka zokwananila zibili zatuntulu, Farao analota. ² Onani, anaimilira mumbali mwa Nailo. Ndipo, onani, ng'ombe zisanu na zibili zinachoka mumumana wa Nailo, zabwino ndipo zoina futi, ndipo zinali kudya muma bango. ³ Onani, ng'ombe zina zokwanila zisanu na zibili zinabwela kukonkapo kuchoka mu Nailo, zoyonda zosaoneka bwino. Beve banaimilila pafupi na ng'ombe zina mumpepete mwa mumana uja. ⁴ Ndipo ng'ombe zosaoneka bwino zija zoyonda zinadya ng'ombe zisanu ndi ziwiri zija zabwino zoina. Pamene apo Farao anauka. ⁵ Anagona futi ndipo analota nafuti kachibili. Onani, ngala zisanu na zibili za tirigu zinamera pa phesi imodzi, zabwino na zabwino. ⁶ Ndipo onani, ngala zisanu na zibili, zofota zo ochewa na mpepo ya kum'mawa, zinamela pambuyo pawo. ⁷ Mitu yofota inamela ngala zisanu ndi ziwili zija zabwino koma futi zozula. Pamene Farao anauka, onani, yanali chabe maloto. ⁸ Ndipo kuseniseni muzimu wake unavutika maningi. Anatumiza kukaitana bamasenga pamozi na banzulu bonse ba ku Aigupto. Farao anabawuza beve maloto yake, koma panalibe wamene anakwanisa kumumangusulila Falao. ⁹ Pamene apo mukulu wa bopelekela chiko anakamba kuli Farao kuti, "Lelo niganizila oa volakwa vanga. ¹⁰ Farao anakalipa na banchito bake, ndipo anani ponya mundende munyumba ya mukulu wa bolonda, ine na mukulu wa bopika buledi. ¹¹ Usiku wamene uja, eve na ine tinalota ali onse kulingana na tantauzo ya maloto yake. ¹² Kwamene kuja tinali pamozi na munyamata wina wachi Heberi, wanchito wa mukulu wa basilikali bolondela mfumu. Tina muuza ndipo anati masulira maloto yatu. Anamasulira ali onse wa pali ise maloto yake. ¹³ Vinachitika monga mwamene anatumangusulira, ndipo vinachiti. Farao ananibweza panchito yanga, koma winangu uja anapachikiwa. " ¹⁴ Pamene apo Farao anatumiza nakumuitana Yosefe. Beve banachita mwa mwachangu naku muchosa mu'ndende muja. Ndipo anagela sisi, nakuchinja vovala, nakungena mwa Farao. ¹⁵ Farao anakamba na Yosefe kuti, Ine ninalota, koma palibe wamene angani mangusulire maloto yanga; koma namvela va iwe, kuti ukamvela chiloto, ukwanisa kumangusula. ¹⁶ Yosefe anamuyanka Farao, kuti, "Sichilii mwa mwa ine. Mulungu azayanka Farao mwadaliso." ¹⁷ Farao ankamba na Yosefe kuti, "Mukulota kwanga ine, onani, ninaimilila mumbali mwa mumana wa Nailo. ¹⁸ Onani, ng'ombe zisanu na zibili zinachoka mumumana wa Nailo, zoina zooneka bwino, ndipo zinadya pakati pa mabango. ¹⁹ Onani, ng'ombe zinangu zinabwela zokonkapo, zofoka, zosaoneka bwino, zoyonda. Ine sininaonepo muziko yonse ya Aigupto zosaoneka bwino monga zija. ²⁰ Ng'ombe zoyonda zosaoneka bwino zija zinadya ng'ombe zisanu ndi ziwiri zoyambilila zoina. ²¹ Pamene zinazidya zija, sizinazibike kuti zinadya, chifukwa zinali zosaoneka bwino monga poyamba. Pamene apo ninauka. ²² Ninayang'ana chiloto changa, onani, ngala zisanu na ziwiri zinamela pa pesi imozi, zozula koma futi zabwino. ²³ Ndipo ona, ngala zina zisanu na zibili, zofota, zoyonda, zoochewa na na mpepo ya kum'mawa, zinamera pambuyo pabo. ²⁴ Ngala zoyonda zija zinamela ngala zisanu ndi ziwiri zabwino zija. Ninauza bamasenga baja, koma panalibe wamene anakwanilisa kunimangusulila ine." ²⁵ Yosefe anakamba kluli Farao kuti, "Maloto ya Farao ni yolingana. Chamene Mulungu afuna kuchita achilangiza kuli Farao. ²⁶ Ng'ombe zisanu na zibili zabwino zija ni zaka zisanu na zibiri, ndipo mitu isanu na ibili yabwino ni zaka zisanu na zibiri. Maloto ayo ni yolingana. ²⁷ Ng'ombe zikazi zisanu na zibili zoyonda zosakondewa zamene zinamela pambuyo pawo ndiye zaka zisanu ndi zibili, ndipo ngala zisanu na zibiri zoyonda zoochewa na mphepo ya kum'mawa zizakala zaka zisanu na zibili za njala. ²⁸ Ichi ndiye chintu chamene ninakamba kuli Farao. Vamene Mulungu afuna kuchita amu langiza Farao. ²⁹ Onani, zaka zisanu na zibili zo chulukila zizabwela mudziko yonse ya Aigupto. ³⁰ Zaka zisanu na zibili za njala zizafika pambuyo pako, ndipo zochulukika zonse zizaka ibalika m'dziko ya Aigupto, ndipo njala izaononga ziko. ³¹ Vochulukila iva sivzazakumbukiliwa muziko chifukwa cha njala yamene izakonkapo, chifukwa izakankala yoyofya kwambili. ³² Chamene chiloto ichi chabwezelewapo kuli Farao nichifukwa chakuti nkani yamene yi yankazikisiwa na Mulungu, ndipo Mulungu azachichita posachedwa. ³³ Manje lekani Farao afunefune muntu wozindikila koma futi wanzeru, amunkazikise eve kunkala olanganila dziko ya Aigupto. ³⁴ Lekani Farao aike boyanganila ziko, ndipo atenge imodzi pa magawo yasanu ya zokolola za mu Aigupto muzaka zisanu ndi zibili zokolola vochulukila. ³⁵ Basonkanise vakudya vonse va zaka vabwino vamene vizabwela ndipo basunge tirigu mumanja ya Farao, inkale yakudya mumi zinda. Bayenera kusunga. ³⁶ Chakudya chamene ichi chizankala chakudya chamu ziko mokwanila zaka 7 za njala yamene izankale muziko ya Iguputo. Munjila yamene iyi ziko si izawonongewa na njala." ³⁷ Magangizo yamene aya yanali yabwino kuli Farao na kuli banthito bake bonse. ³⁸ Farao anakamba kuli banchito bake kuti, "Nanga tingapeze muntu wamene ali monga uyu, wamene muli Mzimu wa Mulungu?" ³⁹ Ndipo Farao anakamba kuli Yosefe kuti, "Popeza kuti Mulungu akuwonesa iwe ivi vonse, palibe winangu wamene niwozindikila nafuti wanzelu monga iwe. ⁴⁰ Iwe uzankala woyanganila nyumba yanga, ndipo monga mwa mawu yako banthu banga bonse bazalamuliwa. Nizankala mkulu kuchila iwe pamupando chabe." ⁴¹ Farao anakamba kuli Yosefe kuti, "Ona, nakunkazika iwe woyanganira ziko yonse ya Igupto." ⁴² Farao anavula mphete yake

yozindikizila kumanja kwake nakuivalika pa kwanja ya Yosefe. Anamuvalika futi vovala va nyula yabwino maningi, ndipo anamumanga na cheni ya golide mumukosi mwake.⁴³ Anamuyendesela mu galeta yachibili yamene anali nayo. Amuna banamu pundila pasogolo pake, "Gwadani pansi." Farao anamuika kunkala woyanganila ziko yonse ya Igupto.⁴⁴ Farao anakamba kuli Yosefe kuti, "Ine ndine Farao, ndipo kuchoselako iwe, palibe muntu wamene azatambasula kwanja yake kapena kwendo yake yake mu ziko yonse ya Igupto."⁴⁵ Farao anaitana Yosefe zina yakuti "Zapenati-Paniya." Anamupasa Asenati, mwana wamukazi wa Potifera wansembe waku Oni, kuti ankale mukazi wake. Yosefe anayenda-yenda mu ziko ya Igupto.⁴⁶ Yosefe anali wa zaka makumi yatatu pamene anaimirira pamaso pa Farao, mfumu ya Igupto. Ndipo Yosefe anachoka pamenso pa Farao, naku yenda yenda mu ziko yonse ya Igupto.⁴⁷ Muzaka zisanu na zibili mwa vochulukila va mu ziko ija vinapakisa mochilapo.⁴⁸ Anasonkanisa vakudya vonse va zaka zisanu na zibili vamene vinali muziko ya Igupto nakusungila vakudya vamene ivi mumizinda. Eve anaika vakudya mumizinda zamene zinali pafupi naminda zamene zinali mumbali mwake.⁴⁹ Yosefe anasunga tirigu munga muchenga wa kumanzi, kufikila mpaka anasiya kupendela, chifukwa vinali vinapakisa kwambili mosakwanisika kupendewa.⁵⁰ Yosefe anali na bana bamuna zaka zibili za njala ikalibe kufika, wamene Asenati mwana wamukazi wa Potifera wansembe waku Oni anamubelekela eve.⁵¹ Yosefe anapasa zina mwana wake woyamba Manase, chifukwa anakamba kuti, "Mulungu andi ibalisa mavuto yanga yonse na banja yanga yonse ya batate banga."⁵² Anapasa zina ya mwana wake wachibili Efulemu, chifukwa anakamba kuti, "Mulungu anibalisa mu ziko ya vovutisa vanga."⁵³ Zaka zisanu na zibili za vakudya vambili vamene vinali mu ziko ya Igupto inasila.⁵⁴ Zaka zisanu na zibili za njala zinayamba, munga mwamene anakambila Yosefe. Kunali njala muma ziko yonse, koma muziko yonse ya Igupto munali vakudya.⁵⁵ Pamene ziko yonse ya Igupto inali na njala, banthu banaitana kuli kuli Farao kuti abapase vakudya. Ndipo Farao anakamba kuli ba Igupto bonse kuti, Endani kuli Yosefe mukachite vamene eve akamba.⁵⁶ Njala inali paliponse paziko yapansi. Yosefe anasegula nkokwe zonse nakugulisa kuli bantu baku Igupto. Njala inakula maningi muziko ya Igupto.⁵⁷ Dziko yonse inali kubwela ku Igupto kugula tirigu kuli Yosefe, chifukwa njala ija inali inafika poipa kwambili paziko yonse yapansi.

Chapter 42

¹ Ndipo Yakobo anaona kuti munali vakudya mu Egipto. Anakamba kuli bana bake bamuna. Cifukwa nichani muyang'ana yang'ana? ² Anakamba, onani apa, namvera kuti kuli vakudya mu Egipto, Yendakoni kuti mukati gulile kuti tinkhale namoyo tisamwalile. ³ Abale bake ba Yosefe bali banayenda kugula vakudya ku Egipto. ⁴ Koma Yakobo sana tume benjamini, mubale wake wa yosefe, pamozi na bale bale popeza anakamba kuti, "Niyopa kuti voipa vingacitike pali yeve. ⁵ Bana ba Israyeli banabwera kugura pakati kabaja banabwera, cifuka njala inali mu ziko ya Kanani. ⁶ Ndipo Yosefe anali bolamulila ziko. Ndipo anali kugulisa kubanthu bonse ba muziko. Abale bake ba Yosefe banafika nakubelama pansi na nkhope zao pansi. ⁷ Yosefe anaona babele bake nakubaziba ana zibisi kuli beve naku kamba nabo mo limba anakamba nao, mwacokela kuti? Banakamba kuli tacokela ku Kanani kubwela kugula vo kudya. ⁸ Yosefe anabaziba ba bale bake, koma beve sibana muzibe. ⁹ Ndipo Yosefe anakumbuka viloto vamene analota pali beve, anakamba nabeve kuti, ndimeneo oipa mwabwela kuona mbali zamene zilibe citezo mu ziko. ¹⁰ " Anakamba kuli yeve kuti, awe mbuye wanga. Ba kapolo bako babwla kugula vakudya. ¹¹ Ndise bana bamunthu umozi tonse, ndife banthu bazoona, bakapolo bako si banthu oipa. ¹² Anakamaba nao kuti, "Awe, mwabwela kuona malo mulibe citeyezo mu ziko ¹³ Bana kamba kuti, "Ife akapolo bako tili abale tyovu, bana bamunthu umozi muziko ya kenani. Ona, mufuna maningi lelo ali nabatate bathu na mubale wathu umozi salimoyo." ¹⁴ Yosefe anababuza kuti, "Ndiye vamene naku uzani. ndimwe oipa. ¹⁵ Pali ici muza yesewa na moyo wa falabo, simuzacoka pario, koma cabe ngati mubale wanu mung'onu abwere kuno. ¹⁶ Tmani umozi mumusiye akatenge mubale wanu. Muzasala mundende, kuti mau yanu yayesewe. Kuona ngati muli cazo ona muli imwe. Ngati siivo, pa moyo wa Falao ndimwe oipa zo ona. ¹⁷ Anaika bonse mundende musiku yatatu. ¹⁸ Yosefe anakamba nabeve pasiku yacitatu, " Citani ici kuti mukhale namoyo, Popeza niyopa Mulungu. ¹⁹ Ngati ndimwe bamuna bazo ona, lekani umozi wa abale wanu akhale mundende iyi, koma imwe mu yende, nyamulani vokodya vanjala ya manyumba yanu. ²⁰ Bwelesani mufana wanu kuti mau yanu ya simikiziwe ndipo simuza mwalila." Ndio banacita zimezo ²¹ Banakambisana wina na muzake, " tinachimwila mubale wathu pakuti tina ona ,kutika kwa moyo wake pamene ana papata kuli ife pamene. anati pempha ndipo sitinamvela, cifukwa caici mavuto yatifikila. cifukwa caici mvuto yatikila. ²² Rubene anabayankha, "Kodi sina kuuzane, Osamucimwila munyamata! Koma sina mvele? Manje onani, magari yake ya funika kwa ife." ²³ Sabanazibe kuti Yosefe anabamwesesa, cifukwa panali omasulila pakati kao. ²⁴ Anacoka pali beve ndipo analila. Ana bwelela kuli beve nokamba nao. Anatenga simiyoni nakumu manga menso yao. ²⁵ Yosefe ana lamulila ba nchito bake kuti ba zuze machola na vakudya, ndikuika ndalama za munthu alibonse mucola cake, ndi ku bapasa vose vofunika paulendo. zinacitika. ²⁶ Abale anasenzesa Abulu ao vakudyandi kuyambapo. ²⁷ Pamene umozi anasegula saka kuti apase bulu zakudya mu malo yopumulila, ana ona ndalama zake. Taonani zinali muku segula kwa thumba yake. ²⁸ Anakamba kuli abale ake, " Ndalama zanga za bwezewamo, zioneni, zili mutumba yanga, "Mitima yanamila anapindamuka monjemela kuyanganana wina na mzake, kukamba kuti, "Nicanici camene Mulungu acita kuli ise?" ²⁹ Anayenda kwa Yakobo, tate wo muziko ya Kanani ndi kumu uza vonse vinaba citikila. Banakamba kuti. ³⁰ Munthu, mbuye waziko, an anakamba, naise moka lipo nakuti ona monga ndise oipa muziko. ³¹ Takamba kuli yeve, ndife bamuna bazona, sindife boipa. ³² Tili abale tyovu, bana ba atate bathu, umozi salimoyo, ndipo ndipo mung'ona lelo ati na batate muziko ya Kenani. ³³ Munthoyo, mwine ziko, anakamba naise, kupitila muli ici nizaziba kuti ndimwe amuna bazo ona. Siyani mubale wanu umozi naine,, tengani vakudya ya njala ku manyumba yanu, ndipo yambaponi. ³⁴ Bwelesani mufana wanu maningi kuli ine. Ndipo nizaziba kuti sindimwe oipa, koma kuti ndimwe bamuna bazoona, Pamenepo ndizatulusa mubale wanu, ndipo muzagulisa muziko." ³⁵ Vinacita pamene anasegula matumba yao kuti, taonani, thumba yalionse munali siliva. Pamene beve naba tate bao banaona mutumba ya siliva, banayopa. ³⁶ Yakobo tate wao anakamba kuli beve, "Mwanitengela bana banga, Yosefe salimoyo, Simioni naye ayenda, ndipo mufuna kutenga Benjamini. Vonse ivi vinthu vaninyamukila ine." ³⁷ Rubene anakamba naba tate bake, kuti, mungapaye bana banga babili ngati siniza bwelesa Benjamini kuli imwe, muakeni mumanja yanga, ndipo ndizaleta kuli imwe futi." ³⁸ Yakobo anati, "Mwana wanga mwamuna sazayenda naiwe, popeza mubale wake anafa ndipo anasala yeka. Ngati voipa vizabwela pali yeve munjira yamene muyendamo, ndipo muzaleta imvi zanga ndicisoni kumanda.

Chapter 43

¹ Njala inapitila mu malo. ² zinacitika pamene bana diya chakudya zamene bana bwelesa ku Igipito, ba tate babo bana kamba ku libeve, "Endani futi, tigulani vakudya." ³ Yudu ana bauza eo. " Munthu monenesa anaticenjeza ife. 'Simuza ona nkhope yanga kufikila mubale wanu ngati ali naimwe.' " ⁴ Ndati muza tituma namubale wathu, tiza enda pasi ndi ku gulalila imwe vakudia. ⁵ Ngati simumutuma eve, citi zaenda pansi, daba uyu munthu anakamba kwaise, simuza ona nkhope yanga pokapo mubale wanu ngatiali naimwe." ⁶ Israeli anakamba, " Chifukwa chani mwani chitila choipa pa kuniuza nyu munthu kuti mulina mubale wanu wina?" ⁷ Bana kamba, " Uyu munthu anati fusa mopitilila zaise ndi banja lathu, ana kamba, ' batate banu balimoyo? Kodi muli na mubale wanu wina?' Tina mu yankha eve kulingana ndi mafuso yake. Sembe tina ziba bwanji zamene aza kamba, 'muletani mubale wanu pasi?'" ⁸ Yuda anakamba kwa Israeli, tate wake. " Mutumeni mwana na ife, tiza yamuka ndi ku yenda kuti ti nkhole moyo ndi kuti ti safe, bose ife, naimwe, ndi oso bana bathu. " ⁹ Niza khala chosimikizilako kwa eve. Muza Muzanipasa muladu ine. Ngati siniza bwaza kwainu kumuonsa pamaso panu, ndipo lekani niyamule dadaulo muyaya. ¹⁰ Angati sitina chedwe, choonadi ziko tawi asembe ti baleko kuno kaci bili." ¹¹ Atate babo Israeli ana kamba kwabeve, ngati cinkhala chocho, maje chitani ici. Tangani zabwino mulomuno mumasaka. Pelekani pasi kwa munthu uyu paso zina baimu ndi uchi. Zonukilisa ndi maya, pistachio nati ndi almondi. ¹² Tenganis dalama mupatikizapo mu manja yanu. Dalama ina bwe zalewa pamene muna segula masaka yanu. Zinyamuleni futi mumaja yanu. Kapena ana sokoneza. ¹³ Tenganiso mubale wanu. Nyamuka ndi ku yendaso kwa munthu uyu. ¹⁴ Lekani mulungu wamphamvu zonse akupaseni imwe chifundo pamaso ya munthu uyu, kwakuti akamulekeleko mubale wanu ndi Benjamani gati nafielewa mwana, na feleawa. ¹⁵ Anthu anatenga paso izi. Ndi mu manja yao antenhga zopatikiza muyeso wa dalama, pamozi ndi Benjamini. Ana nysmuka ndi kuyenda pasi ku Igipito ndi ana imilila kwa Yosefe. ¹⁶ Pamene Yosefe anaona Benjamini pamozi ano, a na kamba kuli osungila nyumba yake." Ba lete banthu munyumba, paya nyama ndi mpika daba banthu bazadya na ine muzuba. ¹⁷ Osunga zamunyumba ya Yosefe ana chita monga Yosefe akambila. Anabaleta kunyumba ya Yosefe. ¹⁸ Aba banthu ba nacita manta chifukwa bana pelekelewa kunyumba ya yosefe. ba na kamba, " Ni chifukwa cha dalama yamene ina bwezelewa muma saka tawi yoyamba tina ikiliwa mukati. Kuti ati sakile mupata motisuzwa ife. Kuti ati mage ise ndi kutitenga akapolo ndi a bulu. ¹⁹ Ana mufikila osunga nyumba ya Yosefe ndi ku kamba naye po lobela munyumba, ²⁰ anati bwana, koyamba ku gula vakudia. ²¹ Zinazinachika, pamene tina fika pamalo tina pumulila tina segula masaka yanthu, ndipo, onani, aliyese pamene tina segula masaka tathu dalama zake zina mumasaka yenze yo kwanila mupimo. tazi bwelesa mumaja yathu. ²² Dalama zina ndiposo tabwelesa mumaja yathu kugula vakudya. Citiziba wamene anti ikila mumasaka yathu." ²³ Osungu anakamba. " Mutendele ukhale na inu. Musa yope. Mulungu wanu ndi Mulungu watate wanu anakufakila moni dalama zanu musaka yanu. Nina ladila dalama yanu." Osunga ana muleta simiyoni kwa beve. ²⁴ Osunga anaba peleka amuna kunyumba ya Yosefe. Anaba pasa manzi, nidipo bana suka medo yabo. Ana pasa zakudya mabulu yao. ²⁵ Bana kozekela paso za Yosefe kubwela kwake kwamu zuba, daba bana vela kuti zadiyela kuja. ²⁶ Pamene Yosefe ata bwela kunyumba, ba naleta paso yamene yanali mumanja munyumba ndi kugwanda pansi. ²⁷ Anaba fusa zaumoyo wao ndi ku kamba. " Ushe batate banu bali cabe bwino, ba chikulile ba mene muna kambapo? Kondi ali moyo?" ²⁸ Bana kamba, " Wachito wanu atate batu bali bwino akali namoyo." Ndipo anamu gwadila kumu chitila ulemu. ²⁹ Pamene ana nyamula menso yake ana ona Benjamini mu bale wake, mwana waba mao make mwamuna. Ndipo ana kamba, " Uyu dye mungono wake wamene una kambapo kuline?" Ndipo ana kamba. " Leka Mulungu aku chitile chisomo kwa iwe mwana wangu mwamuna." ³⁰ Yosefe ana tamanga kuchoka muchibinda, daba china mukwila mutima kwabili kamba kabale wake ana sakila malo kwina kolilila ana enda ku chibinda chake ndi kulila. ³¹ Ana samba kumenso kwake ndi ku cho. Ana zi lesa eve, ku kamba kuti, " Ikani va kuya." ³² Wachito ana konza chakudya cha Yosefe kwa eyeka ndipo abale bake pa beka aku Igoipito ano anadya pabeba chifukwa aku Igipito sanali dyele mukate pamozi nama Hebeli. Kwa ici ni chonyesa ku banthu ba ku Igipito. ³³ Abale bake ana nkhalama pamaso pake Oyamba kubadwa kukonka mwamene bana badwila. Ndipo wa cicepele kuligana na uyamata wake anthu ana dabwisiwa chapamozi. ³⁴ Yosefe anatuma mupimo wazakudia pa songolo pake. Koma Benjamini mupimo unali usanu kupabana a bale ake. Anamwa ndipo bana kondwela na eve.

Chapter 44

¹ Yosefe analamulila wanchito wa munyumba yake, ku kamba kuti, "Zulisa vakudya m' masaka ya bamjuna, kulingana na vamene bangakwanise kunyamula, ndipo ayike ndalama zake aliyense posengula saka yake." ² Uyike kapu yanga, ija ya siliva, pakamwa posegulila saka ya ija mungono paonse, na ndamala yake ya cakudya. "Wanchito wa Yosefe anachita monga mwamene ana mu uzila." ³ Kuseni seni, ndipo bamuna aba banabauza bayende banatenga na ba buru bao. ⁴ Pamene banacoka m'mzinda koma Sbana fike patali maningi. Yosefe anakamba ku wa nchito wake, "Nyamuka, konka ba muna, ndipo ukubapitilila, ubauze kuti, 'Nchifukwa chani mwa bwezela choipa pa cha bwino?' ⁵ Kodi iyi si kapu yamene abwana banga bama mmwela, na kapu yamene ba ma ombezelako? Ichi chintu chamene mwa chita, mwa chita choipa." ⁶ Wanchito anavapitilila na ku bauza mau Mau. ⁷ Bamu uza, "Nichani ba bwana banga bakamba mau monga aya? Ichi chintu chisankale na banchito ku chita cha mutundu uyu." ⁸ Ona ndalama tinapeaza mosegulila masaka yatu, "yamene tinabweesa futi kuli kuchokeku Canani. Manke tingabe bwanji mu nyumba ya ba bwana bako siliva na golide?" ⁹ Ngati aliwonse pali ba nchito bako apezeka nayo, mutekeni amwalile, na ife tizankala ba kapolo ba mfumu wanga." ¹⁰ Wanchito anakamba, Apa manje lekani chinkale monga mau yanu. Wamene azapezeka na kapu azankala kapolo wanga, koma imwe benangu m'mzakala mube mulandu." ¹¹ Kuchoka apo munthu onse anayendesa nakubwelesa nakusitizila saka yake pansi, ndipo aliyense anasegula saka yake. ¹² Wanchito ana sakila. Anayambila mukulu pali onse nakusilizila na mung'ono pa bonse, ndipo kapu inapezeka musaka ya Benjamini. ¹³ Apo bana ng'amba vovala vao. Munthu aliyense anaika katundu yake pali buru nakubwelela ku muzinda. ¹⁴ Yudah na abale nawo, "Nichani chamene mwachita ici? Simuziba kuti munthu monga ine nimachita zo-ombeza?" ¹⁵ Yosefe anakamba, "Tingakambe chani kwa bwana wanga? Tizakamba chani? Kodi tizazilungamitse bwanji? Mulungu aipeza chimo ya mbadwa mubanchito banu. Onani, ndife bakapolo ba bwana wanga, ise namwane kapu yapezeka mumanja mwake." ¹⁶ Yudah anakamba, "Tingakambe chani kwa bwana wanga? Tizakamba chani? Kodi tingazilungamitse bwanji? Muungu aipeza chimo ya mbadwa mubanchito banu. Ona, ndife bakapolo ba bwana wanga, Ise nawamene kapu yopezeka mumanja mwake. ¹⁷ Yosefe anakamba, "Chinkale patali naine cha mutundu uyu kuti ninga chichite, Munthu wamene enze apezeka na kape m'kwanja mwake, uyu munthu anzankala kapolo wanga, koma kwa imwe benangu mutende mwa mtendele kwa atate anu." ¹⁸ Kuchoka apo Yudah ababwela pafupi naye nakukamba, "Mfumu yanga, anapapata lekani wanchito wanu akambeko ku munthu yanu, ndipo mu saleke ukali wanu kuti uyonekele pali kapolo wanu. Chifukwa imwe ni chimodzi modzi na Falao. ¹⁹ Bwana wanga inafunsa banchito bake, kakamba," uli na atate alo m'bale. ²⁰ Tinakamba kwa mfumu, "Tilinayo atate, ba chikulile na mwana wamu ukote wayo muny'ono. Koma mbale wake anafa, ndipo eve aka ndiye anasalapo ya ba mayi bake, na batate bake bomukonda. ²¹ Ndipo munakamba kuli ba chinto banu,, mu bweleseni kiuli ine ni muone! ²² Kuchoka apo tinakamba kuli ba bwana banga, 'Munyamata sangasiye ba tate bake. Ngati abasiya batate bake bazamwalila. ²³ Ndipo munakamba kuli banchito banu, koma chabe mu bwele na m'bela wanu wamung'ono simuzakaona pa menso panga futi. ²⁴ Ndipo chanabwela kuti pamene tinaenda kuli banchito banu atate, tinoba ma ya abwana banga. ²⁵ Atate batu banakamba yendani futi mukatigulile vakudia. ²⁶ Ndipo tinakamba, "Sitinga yendeko khoma ngati, mubale wathu wamung'ono alina ife, Tiza endo, chifukwa chakuti sitizakwanisa kuona pamenso pa uja munthu. Koma chabe nufana wathu ankale naife." ²⁷ Akapolo wanu atate anga analamba kwa ife kuti 'Mu ziba mukazi wanga anabala kuli ine bana ba muna babili. ²⁸ Umodzi ananichoka ine ndipo ninakamba kuti, "Zoonamamujuba juba mu ziduswa duswa, 'kuchika apo sinina muonepo futi. ²⁹ Apa manje mukatenga uyu kuli ine, na choipa chikumu bwelela, muzabwesa pansi imvi zanga na chikwinyilito ku manda. ³⁰ Apa, manaje, nikafika ku wanchito wanu atate, tilibe mung'ono wathu, chifukwa moyo wake wamangila pali muyo wa munyamata uyu. ³¹ Chizachitika akaona kuti tilibe munyamata ife azamwalila. Ba kapolo banu bazabwelasa imvi za kapolo wamu atate mu chisoni paka kumanda. ³² Chifukwa kapolo wanu ine ninakala chisimikizo ca munyamata kuli batate nokamba kuti, ngati sinza bwela nayeve, kuli imwe, apo nizankala wa milandi kwa atate banga tawi zonse. ³³ Kufika apa manje, napapata lekeni wa nchito wanu ankele mumalo mwa munyamata monga kapolo wa abwana banga,, nakuleka munyamata ayende nabale bako. ³⁴ Ningabwelele bwanji kuli atate ngati munyamata sazankala naise? Niyopa kuyenda kuona voipa vinga bwele pali atate banga.

Chapter 45

¹ Ndipo Yosefe anakangiwa kuzileza kuti asalile pa menso pa banchito bake. Anakamba mopunda, "Bonse banisiye," panalibe wanchito aliyense pamene Yosefe anaziulula kuli ba bale bake. ² Analila na chongo, ndipo Aigupto bananvela, na nyumba ya Farao inanvela. ³ Yosefe anati kuli ba bale bake, "Ine ndine Yosefe. Ushe batate banga bakali moyo?" Koma ba bale bake sibanamuyake, chifukwa banali namata pamenso pake. ⁴ Ndipo Yosefe anati uli ba bale bake, "bwelani pafupi naine, napapata." Banabwela pafupi. Anati ndine Yosefe mubale wanu, wamene muna gulisa ku Igupto. ⁵ Osazibalisa na kuzikalipila mweka kuti munaningulisa ine kuno, chifukwa Mulungu ananituma ine pasongolo panu nikapululumuse umoyo. ⁶ Pa zaka zibili izi kwa nkhalajala mumalo ndipo kulinso zaka 5 pamene sikuzankhala kulima kapena kukolola. ⁷ Mulungu ananituma pasongolo panu kuti akakusungeni monga onkhala pa ziko yapansi ndipo kukusungani naumoyo ndi kumasulidwa kukulu. ⁸ Sopano, sindimwe munanituma kuno koma Mulungu, ananifaka kunkhala tate wake wa Farao, bwana wa nyumba yake yonse, ndi olamulila malo yonse ya Igupto. ⁹ Yendesani ndipo muyende kuli batate banga nakubauza kuti, ichi ndiye chamene mwana wanu Yosefe akamba, "Mulungu anipanga ine kunkhala bwana mu Igupto monse. Bwelani kwa ine, ndipo musa chedwe. ¹⁰ Muzankhala mu malo ya Goseni, ndipo muzankhala pafupi naine, imwe na bana banu na bazukulu banu, na nkosa na ng'ombe, na vonse vamene muli navo. ¹¹ Nizakupasani imwe kuja, chifukwa kuli zaka 5 zanjala, kuti musabwele kuumpawi, imwe nyumba yanu, na vonse muli navo." ¹² Onani, menso yanu yaona, na menso ya mubale wanga Benjamini, kuti ndi kamwa kanga kamene kakamba kwa imwe. ¹³ Mukabauze batate banga pa ulemele wanga wonse mu Igupto na vonse vamene mwaona. Muyayendesani kubwelesa batate banga kuno." ¹⁴ Anakumbatila mu'bale wake Benjamini mukosi na kulila, ndi Benjamini analilila mumu kosi wake. ¹⁵ Anapyompyona ba bale bake bonse na kulila kuchoka apo ba bake bana kamba naye. ¹⁶ Nkhani ya ichi chintu inauzidwa kunyumba kwa Farao: "Ba baleba Yosefe babwela chinakondwelesa Farao na ba nchito bake kwambili. ¹⁷ Farao anati Yosefe, "Uza ba bale bako chitani ichi: Longani pa nyuma zanu ndipo muyende ku ziko ya Kanani. ¹⁸ Tengani batate banu na banja ndipo mubwele kwa ine. Nizakupasani vabwino va mu malo la Igupto, ndipo muzadya zonona zamu ziko." ¹⁹ Manje mwauzidwa, 'Chitani ichi, tengani kochikali ku choka mu ziko la Igupto kwa bana banu na ba kazi banu. Tengani batate banu na kubwela. ²⁰ Musaganiza pa vintu vamene muli navo, chifukwa vabwino va ziko ya Igupto nivanu.'" ²¹ Bana ba Israeli bana chita zamene izo. Yosefe anabapasa vi kochikali, monga mwamene anakambila Farao. Ndipo anabapasa vakudya va munjila. ²² Kuli ali bonse anapasa vovala vinangu koma kuli Benjamini anamupasa siliva ili fili handilendi na vovala vili fivi. ²³ Kuli ba tate bake anatuma ivi: Ba bulu bali teni wozula ndi vintu vabwino vaku Igupto; ndi mabulu bakazi bali teni, banatenga tilingu, buledi ndi vinangu vofunika va batate bake vamunjila. ²⁴ Ndipo anabatuma ba bale bake kuti ba yambepo. Anabauza kuti, "Muone kuti musayambane munjila." ²⁵ Bana choka mu Igupto nakubwela ku ziko la Kanani, kwa Yakobo tate wabo. ²⁶ Banamu uza kuti, "Yosefe akali moyo, ndipo wamene alamulila mu ziko yonse ya Igupto." Mutima wake unadabwa, chifukwa sana kulupilile vamene bana mu uza. ²⁷ Bana mu uza mau yonse ya Yosefe yamene ana bauza. Pamene yakobo anaona ma kochikali yamene Yosefe anatuma kumutengelapo, muzimu wa Yakobo tate wawo unauka. ²⁸ Israeli anati, "Zakwana. Yosefe mwana wanga akali moyo. Nizayenda mukumuona nikalibe kufa.

Chapter 46

¹ Isryeli anapanga ulendo navonse ve enze nazo noyenda ku Beresheba. Kuja anapasa sembe kwa Mulungu wa Tate bake Isaki. ² Mulungu anakamba kuli Israeli muchiloto usiku, anakamba, "Yakobo, Yakobo." Ndipo anati, "Nilipano." ³ Anati, "ndine Mulungu, Mulugu wabatate bako. Usayope kuyenda ku Igipito, ndipo kuya nizakupanga ziko yayi kulu." ⁴ Nizayenda naiwe ku igipito, ndipo nizakuleta nafuti ndipo Yosefe azavala menso yako na manja yake." ⁵ Yakobo ananyamuka kuchokella ku beresheba. Bana bamuna ba Israeli banamupeleka Yakobo tate wawo, bana bawo, akazi awo, muchikochikala chamene Farao anatuma kumunya mula. ⁶ Banatenga ngo'ombe zawo na zintu zomwe zebana pindula mu malo ya Kenani. Banabwela ku Igipito, Yakobo nabo badwa mumbuyo mwake. ⁷ Analeta ku Igipito bana bake bamuna naba zukhulu, bana bake bakazi, na ba zukhulu bake bakazi, nabo badwa kumbuyo kwake. ⁸ Aya nimazina yabana ba muna ba Israeli bana bwela ku Igipito: Yakobo nabobadwa kumbuyo kwake, Rubeni, woyambilila kuli Yakobo; ⁹ Bana bamuna ba Rubeni, Hanoki, Palu, Hezroni, na Karmi; ¹⁰ Bana bamuna ba Simeoni, Yamwueli Yamini, Ohadi, Yakini, Zohari, na Sauli, mwana mwamuna wamukazi waku Kanaani; ¹¹ bana bamuna ba Levi, Gerisoni, Kohati na Merai. ¹² Bana bamuna ba Yuda banali Eri, Onani, Sela, Perezi na Zera, (koma Eri na Onani anafa muziko la Kanaani). Bana bamuna ba Perezi panali Hezroni na Hamuli. ¹³ bana banuna ba Issakara banali Tola, Puva, lobi, na Simromi; ¹⁴ Bana bamuna ba Zebuloni banali Seredi, Eloni, na Yaledi. ¹⁵ Aba banali bana bamuna ba leya be anabalila Yakobo mu padaramu, namwana mukazi Dina. Bana bake bamuna naba kazi banali sate fili. ¹⁶ Bana bamuna ba Gadi banali zifioni, Hagi, Suni ezboni, Eri, Arodi, na Areli. ¹⁷ Bana bamuna ba Aseri banali Yimna, Yisiva, na Beriya na Sera we anali mulongo wawo. Bana bamuna ba beriya anali Hederi na Makeli. ¹⁸ Aba ndiye benze ba Zelipa, omwe Labani enze anapasa mwana wake mukazi Leya, aba bana be ana balila Yakobo benzeli Sikisitini. ¹⁹ Bana bamuna bamuka wa Yakobo Rakele banali Yosefe na Benjamini. ²⁰ Mu Igipito manese na Efelemu bana badwa kwa Yosefe kwamukazi Asenati, mwana wa Potifa wansembe waku Oni. ²¹ Bana bamuna ba Benjamini banali bela, beka, Ashibile, Gela, Naamani, Ehi, Loshi, Muppimu, Huppini na Adi. ²² Aba ndiye benenze bana ba Rakele be anabalila Yakobo fotini pamuzi. ²³ Mwana wa Dani enze Hushimu. ²⁴ Bana bamuna ba nafutali banali Jazile, Guni Yeza Shilemu. ²⁵ Aba ndiye bana bamuna ba Yakobo kuli biliha, wamene labani atapasa mwana wake mukazi Rakele seveni pamozi. ²⁶ Onse aba banayenda ku Igipito na Yakobo, banabadwila kumbuyo kwake, kusapendela ko bakazi babana ba Yakobo, banali sikisite sikisi pamozi. ²⁷ Nabana bamuna babili ba Yosefe bana badwila kwa eve mu Igipito, bantu bamu banja lake be bana yenda ku Igipito banali seventy pamozi. ²⁸ Yakobo anatuma Yuda kuli Yosefe kuti amulangise njila yaku Gosheni, ndipo anabwela kumalo ya Gosheni. ²⁹ Yosefe anakonza ngolo yake noyenda muku kumanya Israyeli atate bake kumalo ya Gosheni. Ana bawona, no kumbatila mu mukosi, ndipo analila pamukosi, pantawi yayitali. ³⁰ Israyeli anauza Yosefe, "anje lekani nife, pakuti nawona pamenso pako, kuti ukachili moyo." ³¹ Yosefe anawuza abale ake naba munyumba yaba tate bake, "Nizayenda no uza Farao, kuti, 'Abale anga na ba munyumba yaba tate banga, bamene banali kunkala mumuzinda wa Kenani ba bwela kwayine." ³² Bamuna aba nibosunga mbelele, bankala bo sunga nyama. Baleta mbelele zawo, mbuzi, na zonse zamene bali nazo." ³³ Izafika ntawu pamene Farao azakwitanani no mifunsani kuti, nchito yanu nichani?" ³⁴ Koma mukakambe, 'Banchito banu basunga nyama kuchokela ku bunyamata bwatu kufika manje, ise namakol atu. 'Chitani ivi chakuti munkale mu Malo ya Gosheni, osunga mbelele aliwonse niwonyasa kuli baku Igipito."

Chapter 47

¹ Ndipo Yosefe anangena ndipo anauza Farao, Atate banga na bale bannga, na nyama zabo na zosunga zabo ndi zonse zamene balinazo, bafika kuchokela kumalo ya Kanani. Ona, bali kumalo ya Gosheni." ² Anatenga abale bake bamuna bali feivi ndipo anabazibisa kuli Farao. ³ Farao anakamba kwa abale bake, "Mugwila nchito bwanji?" Bana kamba kwa Farao, "Banchito banu ama onera mbelele, za makolo bantu." ⁴ Ndipo banakamba kuli Farao futi, "Ise tabwela monga alendo muno mumalo. Kulibe zodwesela nyama zabachito bananu, chifukwa kuli njala yopitilila mumalo ya Kenani. Sopano manje, napapata lolani banchito banu kukhale mumalo ya Gosheni." ⁵ Ndipo Farao anakamba kuli Yosefe, kukamba kutii, "Atate bako na babale bako babwela kuli iwe." ⁶ Malo ya Igitipito yali pamaso yanu. Khazikisa ba tate bako ndi babale bako malo kudela ya bwino, malo ya Gosheni ngati uziba bamuna boyenera pakati pao, ubafake otsogolela zobeta." ⁷ Ndipo Yosefe analota Yakobo atate bake na baonesa kuli Farao. Yakobo anadalisa Farao. ⁸ Farao anauza Yakobo kuti, "Kodi wamkhala kwanthawi itali bwanji?" ⁹ Yakobo anauza Farao, "zaka zakuyenda kwanga ni 130 zaka zamoyo wanga ni zing'ono ndipo zobaba. Sizambili ngati zamakolo banga banafa." ¹⁰ Ndipo Yakobo anadalisa Farao na kuchoka pameso yake. ¹¹ Ndipo Yosefe anakhazikisa atate bake ndi abale bake. Anabapasa malo mudziko ya Igitipito, malo opambana, mumdzinda wa Rameses, monga mwamene Farao anakambila. ¹² Yosefe anapasa zakudya atatee bake, abale bake na onse bamunyumba mwabatate bake, kulingana ndi namba ya onse osungidwa. ¹³ Manje kunalibe zakudya mu ziko monse: cifukwa njala yenze yopitilila. Ziko ya Igitipito, na Kanani anaonongeka cifukwa ca mvula osankhalako. ¹⁴ Yosefe anaunjika ndalama zonse zinali mu Igitipito namu Kanani, mogulisa zakidya kubantu. Ndipo Yosefe anapeleka ndalama ku malo ya amfumu Falao. ¹⁵ Pamene ndalama zonse za mu Igitipito na Kanani zinasebenzewa, bantu bonse ba m Igitipito banayenda kuli Yosefe kukamba kkuti, "tipase vokudya! Tizafela cni pamenso yako pakuti ndalama zathu zasila." ¹⁶ Yosefe anakamba kuti, "Ngati ngati ndalama zanu zasila, letani nyama zanu ndipo nizakupasani cakuddya mocinjana na nyama zanu. ¹⁷ Ndipo anabwelesa zosunga zao kuli Yosefe. Yosefe anabapasa cakudy mocinjana na mabulu, nyama siyana-siyana, zosunga zao na madonki. Anabadyesa mukate mocinjana na zosunga zao caka cija. ¹⁸ Pamene chaka china sila, bana bwela kwa ioe chaka chokokhapo ndipo bakamba kwa iye, "Siti zakubisani bwana kuti ndalama zonse zantu ndipo ngombe zonse ndi za bwana wanga kulibe zasalako mumaso bwana, kuchoselako matupi yatu napamene tikhala. ¹⁹ Nichifukwa chani tizafela pameso panu, ise pamozi na dziko yatu? Tiguleni, ndipo ise na dziko tizikhala banchito ba Farao. Tipaseni chakudya kuti tinkale namoyo kuti tisafe, na malo asankhala alibe kantu." ²⁰ Ndipo Yosefe anagulila malo yonse ya Igitipito Farao. Pakuti muntu aliyese wamu Igitipito anagulisa munda wake, chifukwa kunali njala yopitilila. Munjila iyi, malo anakhala ya Farao. ²¹ Kuli bantu, banakhala akapolo bake kuchokela kumalile ena ya Igitipito kufika kumalile kosiliza. ²² Nimalo aba sombe chabe yamene Yosefe sanagule, chifukwa basembe anabapasa zobatandizila. Banadya zobangabila kuchokela kwa Farao zamene anabapasa. Mwaiche sanagulise malo yao. ²³ Ndipo Yosefe anakamba kubantu kuti, "Onani, nagulila Farao imwe na malo yanu lelo. manje izi ni mbeu zanu, zamene muzashanga mu malo. ²⁴ Pa kukolola, mufinika kupasa Farao zachisanu ndipo mbali fo zizankhala zanu, chifukwa mbeu za mumunda ndi za chakudya niza munyumba mwanu nabana banu." ²⁵ Bana kamba kuti, "Wapulumusa umoyo wantu. Tipeze chisomo mumenso yanu. Tizakhala ba chito ba Farao." ²⁶ Ndipo Yosefe ana iyika lamulo yokokhewa mudziko la igipito kufikila lelo, kuti chachisanu chimozi ndi cha Farao. Malo chabe yabasembe niyamene Siyanakhale ya Farao. ²⁷ Ndipo Israeli anakhala mu Igitipito, mu malo ya Gosheni. Batu bake bankhala ndi zintau kumene kuja. Bana paka kwabili. ²⁸ Yakobo anakala mu Igitipito zaka seventini, ndipo zaka za umoyo wa Yakobo zinali handredi foti seveni. ²⁹ Pamene nthawi yakufa kwa Israeli inafika pafupi, anaitana mwana wake Yosefe ndipo anati kuli yeve, "Manje napeza chisomo mwako, ika manja yako pansi pachibelo, ndipo unilagize kukulupilika ndi chilungamo. Napapata osanishika mu Igitipito. ³⁰ Nikagona ndi makolo achimuna banga, uninyamule kunichosa mu igipito naku nishika mu manda yamakolo banga bakudala." Yosefe anati, "Nizachita mwamene mwakambila." ³¹ Israeli anakamba, "Lapa kuli ine," Yosefe analapa kuli yeve. Ndipo Israeli ananguwesa mutu wake pongona pake.

Chapter 48

¹ Ina chitika pa mbofu paizi zintu, umozi anakamba kuli Yosefe, " Ona, atate bako ba dwala." Ndipo anatenga bana bake babili amuna , Manase na Efuraimu. ² Pamene Yakobo ana uziwa, " Ona , mwana wako Yosefe afika kukuona," Israeli ana sakila mphamvu naku nkhalala pa bedi. ³ Yakobo anti yosefe, " Mulungu wa mphamvu anaonekela kuli ine pamalo ya Luz mu Kanaani. Anani dalisa. ⁴ Ana kamba kuli ine, ' Onani, nizaku panga muntu ochuluka, naku kuchulukisa. Niza panga iwe muli maiko Yambili. Niza pasa malo aya kuli bo badwa mu mbuyo mwako na zintu zo yendelela. ⁵ Manje bana bako babili, anabadwa kuli iwe mu Egipto nikalibe ku bwela kuli iwe mu Egipto, ni banga. Efuraimu na Manase ni banga, monga mwamene Rubeni na Simeoni ni banga. ⁶ Bana bamene uza nkhalala nabo kucha abaza nkhalala bako; baza nkhalala bo pendewa ma zina pamozi nabo badiwa nabo potengo zo lobelela. ⁷ Koma pa ine, nika bwela ku choka ku paddani, kulila kwanga Rakele anafa mu malo ya kanaani mu njila, pamene panali mutunda kufika ku Epafra. Ninamu shika kuja pa njila yantu yaku Epafra" (Iyo ni Betelehemu). ⁸ Pamene Israeli anaina mwana wa Yosefe, anati, " niba ndani aba ?" ⁹ Yosefe anati kuli atate ake; " nibana banga, bamene Mulungu anani pasa kuno." Israel anati, " balete kuli ine, kuti ningaba dalise." ¹⁰ Tsopano menso ya Israeli yanali ku lepela chifukwa chau nkhalamba waka, ndipo sanali ku ona. Ndipo Yosefe anaba lefa pafupi nabo, anabafyofyonta nakuba kumbata. ¹¹ Israeli anati kuli Yosefe, " Sininali oyemebekezale kuona pamenso panu futi, koma Mulungu ani vomekeza kuona bana bako." ¹² Yosefe anaba chosa mukati ya mendo ya Israeli, analangana pansi mozichepesa. ¹³ Yose anaba tenga bonse babili, Efuraimu ku zanja la manja kufupi na kwanja ya mazele ya Israeli, na Manase ku kwanja ya mazele kufupi na kwanja ya manja ya Israeli, nakuba leta pafupi na eve. ¹⁴ Israeli anatambika zanja lake la manja naku ika pali Efuraimu pa muntu, wamene anali mufana, na kwanja ya mazele pa mutu wa Manase. Anapapambanisa manja yake, chifukwa Manase anali oyamba ku badwa. ¹⁵ Israeli anadalisa Yosefe, naku kamba ati, " Mulungu wamene atate banga Abrahamu na Isaki, Mulungu wamene anisunga kufika pano, ¹⁶ mungeli wamene anani cingiliza ku vofipi vonse, lekani aba anayamata aba. Lekani zina yanga itanidwe pali beve, na zina yaba tate banga Abrahamu na Isaki. Lekani bakule bochuluka pa ziko la pansi." ¹⁷ Pamene Yosefe anaona kuti atate bake bana ika zanja la manja pa mutu wa Efuraimu sichinamu kondwelese. Ana tenga kwanja yaba tate bake nakuyi vendeza ku choka pa mutu wa Efuraimu kuyi ika pa mutu wa Manase. ¹⁸ Yosefe anakamba kuli atate bake, " Simwamene, atate banga; uyu ndiye wachiyambi. Ikani zanja la manja pa mutu pake." ¹⁹ Atate bake bana kana no yanka, " Niziba, mwana wanga, niziba. Naye aza nkhalala bantu, azankala opambana. Koma uyu mufana azankhala opambanapo kuchila eve, nabo badwa bake bazankala maiko yambili." ²⁰ Israeli anabadalisa ija siku na mau aya. " Bantu ba Israeli baza kamba ma daliso pama zina yanu kuti, 'Ukani MULungu akupanga monga Efuraimu na Manase.'" Muli iyi njila, Israeli ana ika Efuraimu pasongolo pa Manase. ²¹ Israeli anati kuli Yosefe, " Ona, nili pa fupi na kufa, koma Mulungu azankala naiwe, azaku bweza kumalo yaba tate bako. ²² Kuli iwe, monga muntu ali pamwamba paba bale bake, nakupaso chiguli chamene nina tenga kuli ma Amorites na lupanga na uta yanga."

Chapter 49

¹ Pamene apo Yakobo anaitana bana bake bamuna, naku kamba kuti, "Mukumane pamozi, niku uzeni vizakutchitkilani kusogolo kwanu. ² Zi'ikenzi pamozi na kumvelela, imwe bana bamuna ba Yakobo. Nvelelani Isilayeli, tate wanu. ³ Rubeni, ndiwe mwana wanga oyamba, mpamvu yanga, na kuyamba kwa mpamvu yanga, ulemu opambana na mpamvu yopambana. ⁴ Osauzika munga manzi oyenda na mpamvu suzapambana, chifukwa unakwela pa bedi ya batate bako. Pamene unaipisa; unakwela pa bedi panga. ⁵ Simeoni na Levi nipachi bululu. Vida va chongo ndiye mapanga yabo. ⁶ O moyo wanga, usangenemo muchiweruzo chabo; osangenemo mu musonkanonyao, pakuti mutima wanga uli na ulemu ngako pali icho. Pakuti mu ukali wao anapaya bantu, mukukondwela banalemalika ng'ombe. ⁷ Kutembelelamkukalipankwao pakuti wenze oyofya-na ukali wao, pakuti kwenze koipa. Nizabagaba muli Yajoba na kubamwaza mu Isilayeli. ⁸ Yuda, azibululu bako bazakutamnda. Kwanja kwako kuzakankala pamukosi pa badani bako. Bana ba batate bako bamuna bakugwadila pemenso pako iwe. ⁹ Yuda ni mwana wa nkalamu. Mwana wanga mwamuna, wayenda pamwamba kuchoka ku gonjesewa bako. Anabelama pasni, anabendelela munga nkalamu, munga nkalamu ikai, Nindani angayese kumuyimya? ¹⁰ Nkoli yau mfumu siyizakachoka pali Yuda, kapena cholamulila pakati pa mendo yake, mpaka shilo akabwele. Maziko yazamunvelela. ¹¹ Kumangila bulu wake ku mpesa, na mwan wa bulu wake pa mpesa osankiwa, A'washa vovala vake mu moba, na mukanjo wake mu magazi ya mpesa. ¹² Mu menso mwake bazakankala wofipa mong ni niyu, na meno yake kuyela munga ni mukaka. ¹³ Zebuloni azankala kumbali kwa nyanja. Azankala pofkila pa ma bwato, na malile yake yazafika ku Sidoni. ¹⁴ Isaka ni bulu wolimba kugona pakati pa mogona mbelele. ¹⁵ Aona alo bwino opumulilamo na malo okondwelesa. Azagwesa pewa yake kukatundu na kunkala kapolo wa nchtio. ¹⁶ Dani azakaweluza bantu bake munga wa mitundu ya Isilayeli. ¹⁷ Dani azakanla njoka mbali mwa mseu, nkokka yoipa munjila yamene iluma ku mendo kwa bulu, kuti okwelapo amagwela kumbuyo. ¹⁸ Nizaymbekeza chipilumuso chanu, Yehova. ¹⁹ Gadi-vigabenga vizamumenya, koma azabamenya ku mendo kwao. ²⁰ Vokudya va Asha vizakankala vabwino, ndipo azapeleka vonona ku ufumu. ²¹ Nafitali ni ka nyama komasuka, apa mau abwino. ²² Yosefe ni msambo obala, Mutengo obala mbali mwa manzi, yamene misambo yake misambo yake ikwela pamwamba pa chiumba. ²³ Badani bake bazamumenya na kumulasa na kumuvuta. ²⁴ Koma cholasila chake chizankala cha mpamvu, na manja yake yazalimbikisiwa chifukwa cha zina mbusa, mwala wa Isilayeli. ²⁵ Mulungu wa batate bako azakutandiza na Mulungu wa mpamvu azakudalisa na madaliso ya kumwamba, madaliso yoyendelela pasni pa manzi, na madaliso ya maziba na mumala, ²⁶ Madaliso ya batate bako nibopambana kuchila madaliso ya kudala olo vintu yokumbukila va kumalupil yang'ono ya kudala. Lekani yankale pamutu pa Yosefe, nangu pa kolona ya pa mutu pa mwana mwamuna wa mfumu ya abululu bake. ²⁷ Benjamini ndiye galu yamsanga yanjala, mumawa azadya na muzulo." ²⁸ Aya ndiye mitundu twelofun ya Isyalei. Ichi ndiye chamene anakamba batate bao pamene anabadalisa. Alyense anamudalisa na madaliso yake. ²⁹ Pamene anabalangiza benve na kukamba kuli benve, "Nili pafupi kuyenda kuli bantu banga. Mukanishike na makolo bana mankwema chili mu munda ya Efroni mu Hititi, ³⁰ Munkwema ili mu munda wa makipela, ili pafupi na mare mu malo ya Kanani, malo yamene Abrahamu anagula kwa Efroni Hititi kuti ankale manda. ³¹ Kuja banashika Isaki na Rabeka mukazi wake; ndipo kuja ninshika Leya. ³² Munda na nkwema yamene vilimo vinguliwa ku bantu baku Heti." ³³ Pamene Yakobo pamene anasiliza malandizo aya ku bana bake, anadonsela mendo yake pa bedi, ma kupema kosilizila, nakuyenda kuli bantu bake.

Chapter 50

¹ Ndipo Yosefe ana lemesedwa kwa kuti anagwa pa nkhope yake ba tate. Ndipo anamulilila eve, ndipo ana mu fyofyonta. ² Yosefe ana lamilila a dotolo ba chito bake ku konza tupi ua tate bake. Sopano a dotlo ana konza Isreali. ³ Bana tenga masiku fote, pakuti inanli ntawi yakwanila kwakuti amukonze. Ba ku Egipito analila masiku okwanila seventi. ⁴ Pamene masiku olila ana sile, Yosefe anakamba ku nyumba ya Falao, anakamba, "ngati manje napeza mwai mu meso yako, napapata nikambileni kuli Falao kukamba kuti." ⁵ Ba tate banani Lepisa kukamba, "Ona nili pa fupi kufa. Ne shikeni mu manda mwamene niza zikumbila ine neka muziko ya Kenaani. Ukudiye muzanishika ine." Manje lekani ine niyende nika shike ba tate banga. Ndiponso nizabwelela. ⁶ Falao anayanka, "Enda ka shike ba tate bako ba, banani lapisa." ⁷ Yosefe ana yenda ku ka shika atate bake. Ba nchoti bonse ba Falao bana yenda na eve bakulu bakulu bonse muyumba yake. Bonse bamu ziko la Egipito, ⁸ na nyumba yonse ya yosefe ndi abale bake bonse, ndipo ba munyumba yabatate bake. Koma bana babo, Vobeta kabo, ndi ngobe zao zina sala mu malo ya Gosheni. ⁹ Golo ndi aka valo zina yenda beve cinali cigulu cacikulu cabanthu. ¹⁰ Pamene bana bwela ku malo yopepeptela ya Atadi kumbali ina ya Yolodani, ana lilila kwakululu movesa chifundo. Uku Yosefe ana panga ma siku asanu ndi ziwili kulila ba tate bake. ¹¹ Ndipo onkhala mu ziko amu Kenaani, anaona kulila pasi ya Atadi, bana kamba, "Ici ni cisoni cacikulu kwa banthu ba ku Egipito." Chifukwa cake malo a itaniwa Abeli Mizraimu kupitilila Yodani. ¹² Sopano bana bake ba Yakobo ana chita zamine ana ba lamulila beve. ¹³ Bana bake bamuna anamunyamula eve ku malo ya Kenaani ndi kumshika muci kwema mumunda wa machipela pafupi na Mamri. Abrahamu ana gula mukwema ndi munda malo yo shikilako. Anagula kwa Efuraimu ma Hititaiti. ¹⁴ Pambuyo yo shika ba tate bake. Yosefe ana bwelelela ku Egipito. Eve, pamozi na abale bake ndipo bonse ana mupelekeza eve mu shika ba tate bake. ¹⁵ Ndipo abale ba Yosefe pamene bana one kuti ba tate babo bafa, bana kamba manja ngati Yosefe akati nkhalila naukali ise ndipo nakufuna kytibweza ise zoipa zose tina chita kwa eve? ¹⁶ Sopano bana lamulila ku pezekapo kwa Yosefe. kukamba kuti, "Ba tate banapasa malamulo bakelebe kufa kukamba, ¹⁷ Uzeni yosefe izi," napapa ba kukukila abale bako machimmoyabo ndi zolakwa zawo pamene bana chita zoipa kuli iwe." Manje napapata ba kukukile ba tumiki ba Mulungu ba batate bako." Yosefe analila pamene bana kamba na beve. ¹⁸ Ba bale bake futi ana yenda ndi kugona choyangana pasi pamaso pake. Bana kamba, "One, ndise ba nchito bako." ¹⁹ Koma Yosefe ana bayanka beve, "Musayope. kodi nilimumalo ya Mulungu?" ²⁰ Kwa iwe, munanifunila zoipa ine. Koma ana ni funila zabwino. Ku pulumusa miyo zaanthu ambili. Monga muona lelo. ²¹ Manje musayope nizakupasane vintu iwe na bana bangona anabalikisa beve munila yambwinno akukamba zabwino ku mitima yabo. ²² Yosefe ana nkhalila mu Egiito, pamozi na banja yaba tate bake. Ana nkhalila zaka 110. ²³ Yosefe ana ona bana ba Ephraimu na bana bana badwa mumubada wachitatu, ndiposo ana ona bana ba Makira aba ba Muna ba Manase, ba mane ba Fakiwa pama nkhonkhola ya Yosefe. ²⁴ Yosefe ana kamba kwa abale bake, "Nalipa fupi kufa, koma Mulungu zoonza azabwela kwa imwe na kuku sogolelani kuku chosa mu malo yamene ana lapa ku pasa Abram ku Isaki ndi Yakobo. ²⁵ Ndipo Yosefe ana panga bana ba muna ba Israeli kulapila pangano, "Mulungu chazoonza aza bwela kwa inu. Patiwe ija mufunika muka yamule ma boza yanga kuyta chosa muno." ²⁶ Sopano Yosefe anafa, na zaka 110 bana koza tupi yake ndi po ana ika mu bokosi ku Egipito.

Exodus

Chapter 1

¹ Aya ndiye ma zina ya bana ba Izilayeli bamene banabwela mu Igupto pamozi na Yakobo, ali onse na banja yake: ² Lubeni, Simiyoni, Levi, na Yuda, ³ Isaka, Zebuluni, na Benjamini, ⁴ Dani, Nafutali, Gad, na Asha. ⁵ Bonse bantu pamozi bamene banali mubadwe wa Yakobo banali 70 kubapenda. Yosefe eve anali ku Igupto kudala. ⁶ Yosefe, babale bake bonse, na uja mubadwe wonse unamwalila. ⁷ Bana ba Izilayeli banali bana nkala na bana bambili, nafuti banankala bakali; ziko yonse banali bana zula. ⁸ Manje kunayamba kulamulila mfumu inangu mu Igupto, yamene si inali kuziba kali konse pali Yosefe. ⁹ Anauza bantu bake kuti, "Onani, ba bantu ba Izilayeli bapaka maningi nafuti bali na mpavu kutichila ise. ¹⁰ Bwelani, tiyeni tiba bele nzelu, ndaba bazapitiliza ku paka, futi ngati kwankala nkondo, baza nkala pamozi na badani batu, nakuyamba kumenyana naise, nakutaba muziko." ¹¹ Mwai ichi baika boba langanila pa ntchito kuti bakazibavuta muku bapasa ntchito zokosa. Ba Izilayeli bana manga mizinda za Falao: Pitomu na Lamesesi. ¹² Koma mukulingana na mwamene banali kubavutisila kuli ba Igupto, ndiye mwamene ba Izilayeli banali kuchulukila nakuzula mu ziko yonse. Mwamene umu ba Igupto

banayamba kuyopa bantu ba mutundu wa Izilayeli.¹³ Ba Igupto bana yamba kulengesa kuti bana ba Izilayeli kuti bayambe kusebenza na mpoavu.¹⁴ Bana panga myoyo zabo kunkala zobaba chifukwa cha kulimba kwa ntchito za malibwe na daka, na mu zintchito zonse zamu minda. Ntchito zamene banali kufunika kutchita zibnali kufuna kusebenza mwa na mpavu.¹⁵ Chokonkapo mfumu waku Igupto anakamba na botandizila azimai ponkala na bana; umozi zina yake inali Shipula, na wina Puwa.¹⁶ Anabauza kuti, "Pamene imwe mutandizila bazimai bachi Hebeli paku nkala na bana, mukaziyanganisisa pamene bankala na mwana. Ngati mwana ni mwamuna, imwe mufunika kumupaya; koma ngati nimukazi, nikumusiya."¹⁷ Koma baja bazimai banali bantu boyopa Mulungu sibanachite mwamene mfumu ya Igupto inabauzila; koma, banaba lekelela bana bamuna na moyo.¹⁸ Mfumu yaku Igupto inaitana baja bazimai botandizila ponkala nabana naku bauza kuti, "Kansi nichani chamene mwachitila ichi, kubalekelela bana bamuna kunkala namoyo?"¹⁹ Bazimai banamuyanka Falao kuti, "Bazimai bachi Hebeli sibali monga bazimai bachi Igupto. Bali na mpavu bama nkala na mwana ise pamene tikalibe nakuyamba kuba tandizila."²⁰ Mulungu anabachingilizila aba bazimai. Bantu banapaka nafuti banankala na mpavu.²¹ Chifukwa chakuti bazimai aba banali boyopa Mulungu, anabapasa na banja yabo.²² Falao anauza bantu bake bonse kuti, "Muyenela kuponya mwana mwamuna ali onse wamene abadwa mu nyanja, koma mwana mukazi ali onse muyenela kumusiya na moyo."

Chapter 2

¹ Manje mwamuna wamutundu wachi Levi anakwatila mukazi wachi Levi. ² Mukazi anakala namimba naku bala mwana mwamuna. Pamene anaona kuti anali mwana mwaumoyo wabwino, anamubisa myezi itatu. ³ Koma pamene analeka kumu bisa kumubisa, anatenga basiketi ya papiras, naku mata na bituman na ulimbo. Manje anamufakomo mwana mukati nakufaka pama tete mumanzi. ⁴ Mulongo waka anaimilila patali kuti aone vizachitika kuli enve. ⁵ Mwana mukazi wa Farao anabwela kusamba kumanzi apmene bosenza bake benze kuyenda mumbali mwa manzi, anaona basiketi pakati pa tete naku tuma banchtio bake baitenge. ⁶ Pamene anaisegula, anaona mwana. Onani, mwana anali kulila. anankal nachifundo pali enve naku kamba, "Uyu zo'ona nimwana waumozi wama Heberi." ⁷ Koma mulongo waka mwana anuza mwana wa Farao, "kodi niyende kusakila mukazi wachi Heeri wamene azayamba kusunga mwaa uyu?" ⁸ Mwana mukzai wa Farao abaumza iye, "Yenda." naku kamusikana kangono kanayenda nakutenga bamai bake ba mwana. ⁹ Mwana mukazi wa Farao anauza bamai ba mwan, Tenga mwana uyu uninyosheleko, ine nizakulipila." Pamene mukazi anamutenga naku munyosha. ¹⁰ Pamene mwana anakulako, bana muleta kuli mwana mukazi wa Farao, anso anankala mwana wake. Amamupasa zina ya Mose naku kamba, "chifukwa ninamu chosa mu manzi." ¹¹ Pamene Mose anakula, anayenda kunja kubantu bake anaona kusebenza maingi kwao. Anaona mu Iguputo anmenya bantu bake. ¹² Analangana uku kumbali na uku kumbal, koma pamene anaona kuti kunalibe aliyense, Anapaya mu Iguputo naku bisa tupi yake mu michenga. ¹³ Anachoka siku yokankapo, na, onani, bamuna babili ba chi Heberi benze kumenyana. Anauza umzi wamne enze olakwa, "Nichani chamene umenyala muzako?" ¹⁴ Koma mwamuna anamu'uzi, "nindani akupanga mukulu na otiweluzi pali ise? Nanga uganiza kunipaya ine munga mwamene unaoaila mu Iguotuo?" Pamene apo Mose anankala na manta anakamba, "vamene nina chichita zo'ona vazibika kuli benangu." ¹⁵ Koma pamene Farao anavela pali ichi, anayesa kupaya Mose. Koma anamutaba Farao naku nkala ku ziko yaku Midani. Kuja anakankala pansu pa mbali ya chisime. ¹⁶ Manje wansembe waku Midani anali nabana bakazi bali seveni. Bana bwela, kutapa manzi, nakmunfaka muvotapila manza kuti bamwese nyama zosunga. ¹⁷ Bobetela bana bwela naku yesa kuba pisha, koma Mose anayenda naku batandiza. Pamene apo anaba mwesela nyama zosunga. ¹⁸ Pamene basikanaka banayenda kuli Reueli atate bao, anakamba, "nichani mwabwela kunyunmba musanga lelo?" ¹⁹ Bana kamba, "waku Igiuputo atipulumusa ise kuli mbusa. Ati tapilana manzi naku mwesa nyama zosunga." ²⁰ Anabauza bana baka bakazi. "Nanga alikuti? nichani mwamusiya mwamuna? Muitaneni kuti adye chakudya naise." ²¹ Mose anavomela kunkala na mwamuna, wamne futi anamupasa Zipora mwana wake mukazi kuti akwatile. ²² Anabala mwana mwamuna, na Mose anamupasa zina Geshomu, yachilendo." ²³ Pamene kunapita ntau, mfumu yaku Iguputo inafa. Ba Isilayeli banalila chifukwa chanchito yaukapolo. Bana lila kufuna tandizo, naku pempa kwao kunayenda kuli Mulungu chifukwa chaukapolo. ²⁴ Pamene Mulungu anavela kulila kwao, Mulungu anakumbukila pangano yamene inali pakati pa enve na Abrahamu, Na Isaki, na Yakobo. ²⁵ Mulungu anabaona bana ba Isilayeli, naku ziba kuvutika kwabo.

Chapter 3

¹ Manje Mose anali akali kubusa vobeta va Yotero mu pongozi wake, wansembe wa Midiyan. Mose anasogolela vobeta ku mbali. yakutali ya chipululu anafika pa Horebu, lupili Mulugnu. ² Kwamene uko Mungelo wa Yehova anaonekela kuli enve muchi mbili-mbili chamulilo musanga. Mose anayangana, ndipo onani, musanga unali kubuka, koma chisamba sichenze kunyeka. ³ Mose anakamba, "nizapatukila kumambali kuti ni one ichinchintu chodabwisa, chifukwa ni chani chisamba sichinyeka." ⁴ Pamene Yehova anaona kuti anapatulila pa mbali kuyangana, Mulungu anamuitana kuchokela muchisamba na kukamba, "Mose, Mose." Mose anakamba kuti, "nili pano." ⁵ Mulungu anakamba kuti, "osabwela pafupi! Vula nsapato zako ku mapzai yako, Chifukwa pamalo apa pamene waimilia ni popatulika kuli ine." ⁶ Anaikapo, "Ndine Mulungu wa batate bako, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isaki, na Mulungu wa Yakobo." Pamene apo Mose anazivininkila ku menso, chifukwa anayopa Mulungu kuyangana Mulungu. ⁷ Yehova anakamba, "Naona zo'ona kuvutika kwa bantu banga bali mu Iguputo, namvela kulila kwao chifukwa chabantu bobasebenzesa, chifukwa zakutika kwao." ⁸ Naseluka pasni kuba masula kuchokela ku mpavu zama Iguputi na kubaleta mumalo ya bwino, malo yakulu, kuziko ya mukaka na uchi ku malo yaku kanani, Ahiti, Aamol, Aperz, Aperizi, Ahivi na Ayebusi. ⁹ Manje kulila kwa bana banga kwafika kuli ine, ndiponso, naona kutiiliziwa kwawelesawa nama Iguputo. ¹⁰ Manje apa, Nizakutuma kuli Farao kuti ubwelese bantu banga, ba Isilayeli, kubachosa mu Iguputo." ¹¹ Koma anakamba kuli Mulungu, "Ndine ndani ine, kuti niyende kuli Farao naku bwelesa bana ba Isilayeli kubachosa mu Iguputo?" ¹² Mulungu anayanka, nizamkala naiwe nditu. Ihci ndiye chamene uzabilako kuti ine nakutuma. vikachosa bantu mu Iguputo, uzaniyamika in pa lupili ino." ¹³ Mose anakamba kuli Mulungu, "Pamene nizayenda kuli ma Isilayeli na kubauza. Mulungu wa makapolo anituma kuli imwe," ndipo baka kamba kuli ine, zina yake nindani? nichani chamene nizakamba? ¹⁴ Mulungu anakamba kuli Mose, "INE NDINE MWAMENE NDILILI." Mulungu anakamba, ufunuka kukamba kuli ba Isilayeli, INE NDINE anituma kuli iwe. ¹⁵ Mulungu anakambanso kuli Mose ufunika kukamba ku Isilayeli, 'Yehova, Mulungu wamakolo yanu, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isaki ndi Mulungu wa Yakobo, anituma kuli iiwe. Iyi ndiye zina kumbukiliwa na mibadwo yonse. ¹⁶ Yenda ulongane bakuluvbonse bamu Isilayeli pamozi. Kamba nabo kuti, Yehova, Mulungu wa makolo, , Mulungu wa Abrahamu, Isaki ndi Yakobo, aonekela kwaine naku kamba, "nankala ninyang'ana ndipo naona vamene vachitika kuli imwwe mu Iguputo. ¹⁷ Nalonjeza kukuchosani mumalo ya botitiliza mu Iguputo kukupelekani kumalo yaku kanakni, Ahiti, Aamori, Aperizi, Ahivi na Ayebusi, muziko yoyendamo mukaka na uchi." ¹⁸ Bazakumvelelani imwe. Iwe na bakulu bamu Iguputo, ndipo mufunika ku mu'uzi, .Yehova, Mulungu wa Aheberi, akumana naise. Manje tiyende uledno wa masiku yatatu muchipululu, kuti tikapeleke nsembe kuli Yehova Mulungu watu. ¹⁹ Koma niziba mfumu yaku Iguptuo sizakuleka ni kuti muyende, koma chabe kukakamiza kwanja yake. ²⁰ Nizatambasula kwanja yanga na kumenya ma Iguputo navo dabwisana vonse pake azakulekani. ²¹ Nizapasa aba bantu mwai pamenso yama Iguputo, chakuti mukachoka , simuzayenda mulibe chili chonse. ²² Muzimai alionse azafunsa siliva na golide vokomesela vovalika kuchoka kuli bantu bake bamu Iguptuo na bazimai bankala mu manyumba yapafupi. muzavi ika pali bana banu bamuna na bakazi, munjila yiy muza ononga ma Iguputo."

Chapter 4

¹ Mose anayanka, nanga ngati sibazani kulupilila olo kunimvelela koma benve kukamba, Yehova sana onekela kuli iwe?" ² Yehova anakamba kuli enve, nichani chili mu manja mwako? Mose anakamba, "nkoli." ³ Yehova anakamba kuti, "Iponye pansi." Mose anaiponya pansi, naku sanduka njoka. Mose anatabila kumbuyo. ⁴ Yehova anakamba kuli Mose Kuti, "Tambusula kwanja uyigwile kumuchila." Chakuti anatambulusa nakuyigwila njoka. Inankala futi nkoli mumanja mwake. ⁵ "Ivi vili chakuti ba kulupilile kuti Yehova, Mulungu wa makolo yao, Mulungu wa Abrahamu, Isaki ndi Mulungu wa Yakobo aonekela kuli iwe." ⁶ Yehova anakamba kuli enve, "Manje apa faka kwanja yako mu chovala chako, "Ndipo Mose anaika kwanja kwake mu chovala futi." Pamene anaichosa, onani, kwanja kwake kunali namakate yoyela monga matalala. ⁷ Yehova anakamba kuti, "faka kwanja yako mu chovala futi, "Ndipo Mose anaika kwanja yake mu chovala futi." Pamene anaichosa, anaona kuti ya nkala bwino futi, monga tup yonse. ⁸ Yehova anakamba kuti, "ngati sibana kulupilile iwe-ngati sibanaku fakeko nzelu kuchi zindikilo choyamba champamvu zanga olo ku kulupilila pamene apo bazakulupilila chachibili. ⁹ Ngati sibazakulupilila ngakale ivi vizindikilo vibili va mpamvu, olo kumvela kuli iwe, pamene apo tenga manzi ya mumana nakutatila pa doti yoyuma. ,anzi yamene uzatenga yaza sanduka magazi pa doti yoyuma. ¹⁰ Pamene Mose anakamba kuli Yehova kuti, "Ambuye" nikalibe kukambapo bwino, kapena kudala olo kapena mwamene muna kambilapo nayenve kapolo wanu ndine wachibwibwi na lulimi yanga niyolem." ¹¹ Yehova anakamba kuli enve, nindani anapanga kamwa yamuntu? Nindani anapanga mu tu kuti asakambe olo asakame olo ayangane olo aleke kuyangana? kodi sindine, Yehova? ¹² Manje yenda, nizankala na kamwa kako na ku kupunzisa vamene ufunika kukamba." ¹³ Koma Mose anakamba, "Ambuye, napapata tumani alionse wamene mu ngafune kutuma." ¹⁴ Koma Yehova anakalipa na Mose. Anakamba, "Nanga Aroni, mubale wako, mu Levi? Niziba kutianga kambe bwino. Komanso, abwela kukumana naiwe, ndipo akaona iwe, aza kondwela mumutima mwake. ¹⁵ Uzakamba nayenve nakufakamo mau yokama mukamwa mwake. Ine nizankala na kamwa kako na kamwa kake, ndipo niza kuonesani mose vochita. ¹⁶ Ndiye azaku kambilako kuli bantu. Azankala kamwa kako. Ndipo uzankala kuli enve monga ine, Mulungu. ¹⁷ Uzatenga mumanja mwako nkoli iyi. Nayenve uzachita zizindikilo." ¹⁸ Pamene apo Mose anabwelela kuli mupongozi wake Yetelo naku kamba naye. "Nilekeni niyende nibwelele kuli babululu banga bali ku Iguputo nione ngati bakali namoyo." Yetelo anakamba kuli kuti, "Yenda mu mutendele." ¹⁹ Yehova anakamba kuli MOse mu Mdiyani, "Yenda, bwelela ku Iguputo, chifukwa bonse bantu benze kufuna kutenga moyo wake banafa." ²⁰ Mose anatenga bakzi bake na bana bake na kubaika pa bulu. bwelela kuziko la Iguptuo, ndipo ananyamula nkoli ya Mulungu mumanja mwake. ²¹ Yehova anakamba kuli MOse kuti, "Pamene uzabwelela ku Iguputo, ona kuti uchite pamenso ya Farao vonse vodabwisa vamene baika mu mpamvu zako. Koma nizza kosesa mutima wake, ndipo sazaleka bantu bayende. ²² Ufunika kukamba kuli Farao, 'Ivi ndiye vamene Yehova akamba: Isilayeli ni mwana wanga mwamuna, mwana wanga oyamba. ²³ ndipo nikamba kuli iwe, "Leka mwana wanga mwamuna ayende, chakuti akaniyamike." Koma chifukwa wakana kumuleka kuti ayende, ni zapaya mwana wako, mwana oyamba wako mwamuna." ²⁴ Manje munjila, pamene banaimilila usiku, Yehova anakumana Mose nakuyesa kumupaya. ²⁵ Koma Zipola anatenga mupeni wamwala na kujuba nyama ya mwana wake mwamuna, naku igwilisa kumendo yake. Nakukamba, "Zo'ona iwe ndiwe mukwati wanga wama magazi kuli ine." ²⁶ Pamene apo anamulekelela eka. Anakamba, ndimwe mukwati wanga wama magazi chifukwa chamudulidwe. ²⁷ Yeho a anakamba kuli Aroni, "Yenda muchipululu uka kumane na MOse." Aroni anayenda, anakumana naye palupili ya Mulungu, na kumu pyopyonta. ²⁸ Mose anauza Aro i mau yonse ya Yehova yamene anamutuma kukamba pali zizindikilo za mpamvu zamene anamula mulila enve kuchita. ²⁹ Pamene apo Mose na Aroni banayenda nakuika pamozi bakulu bonse bamu Isilayeli. ³⁰ Aroni anakamba mauyonse yamene Yehova anakamba kuli MOse. Anaoselanso zizindikilo va mpamvu ya Yehova mu muenso ya bantu. Bantu bana kulupilila. ³¹ Pamene bana mvela kuti Yehova ayangana ba Isilayeli na kuona kutitiliza kwao, pamene benve banagwada pansi naku muyamika.

Chapter 5

¹ Pamene ivi vintu vibachita, Mose na Aroni bana yenda kuli Farao nakukamba kuti, "Ivi ndiye vamene Yehova, Mulungu wa Isilayeli, akamba: 'Leka bantu banga bayende, kuti bakachite pwando muchipululu.'" ² Farao anakamba, "Yehova nindani? Nichani chamene nizabanvelela kuti niba leka bayende? Sinimuziba Yehova: Sinizaleka Isilayeli kuyenda" ³ Banakamba, "Mulungu waba Hebeli atikumanya ise. Lekani tiyende pa ulendo wama masiku yatatu muchipululu na kupelka nsembe kuli Yehova mulungu kuti asabwelese pali ise chilango olo mukondo." ⁴ Koma mufumu ya Igiputo inakamba kulibe, "MOse na Aroni, nichaninmuchos bantu panchito yao? bwelelani pa nchito yanu." ⁵ Anakamba futi, "Manje mulibantu bambili mumalo yatu, anso ulekengesa kuti baleke nchtio yao." ⁶ Pasiku yamene ija, Farao anapeleka lamulo kuli mabwana bakulu nabo onelela nchito ku bantu. Anakamba, ⁷ "Kusiyana nakudala, Osabapase bantu uzu paku panga ma buloko. Baleke bayenda kuzitengela mauzu paboka." ⁸ Koma, mupitilze kubauza kuti bazipanga nambala yama buloko kulingana na yamene banali kupanga kudala. Osavomela chilichonse chachepa apo, chifukwa bali naulesi. Nichifukwa chake bali kuitana na kukamba, Tileke tiyemde anso tikapeleke nsembe kuli Mulungu watu." ⁹ Ikilaponi nchito yao amuna kuti bapitiliza kukamba na osaikilako nzelu ku mau yao yabo." ¹⁰ Pamene apo bakulu ba nchito na bamuna boyanganila bantu bana yenda naku bauza bantu. Banakamba, "Ivi ndiye vamene Farao akamba: Sinazakupasani imwe mauzu." ¹¹ Imwe mweka muzafunika kuyenda naku zitengela kwamene munga ipeze, koma nhito yanu siyiza chepesewa." ¹² Pamene apo bantu bana salangana pa malo yonse ya Iguputo ku'unjika mauzu. ¹³ Bakulu ba nchito banapitiliza kubalimbisa naku kambakuti, "Silizani nchito yanu, monga mwamene munali kusilizila pamene mauzu yanali kupasiwa kuli imwe." ¹⁴ Bakulu ba nchito ba Farao bana menya boyanganila ba nchito bama Isilayeli, bamene baja banafakiwa kuyanganila ba nchito. Bakulu ba nchito banapitiliza ku bafunsa, "Nichani simuna pange yonse ma buloko yamene mufunikila kupanga, siku yapita na lelo, monga mwamene mwenze kuchitila kudala?" ¹⁵ Manje boyanganila nchtio bana bwela kuli Farao na kulila kuli enve. Banakamba kuti, "nichani chamene mutisungila monga ivi ba ncbito banu?" ¹⁶ Kulibe mauzu yapasiwa kuli ba nchito banu, koma bakali kuti uza ise, 'pangani ma buloko!' Ise, ba nchito banu, bamenyewa manje, koma nivuto ya bantu bako." ¹⁷ Koma Farao akamba kuti, "Muli na ulesi! Ukamba kuti! Tivomeleseni kupeleka nsembe kuli Yehova." ¹⁸ Manje apa bwelelani kusebenza. kulibe mauzu yazapasiwa kuli imwe, koma mufunika kuipanga nambala yama buloko yamene ija." ¹⁹ Oyanganila nchito baku isilayeli anona kuti banali mubvuto pamene banauziwa, "Simufunika kuchepesa nambala yama buloko pasilu." ²⁰ Banakumana Mose na Aroni, bamene banali kuimilila panja panyumba ya mfumu, pamene banali kuchoka kuli Farao. ²¹ Banakamba kuli Mose na Aroni, "Lekani Yehova akuone iwe naku kulanga iwe, chifukwa walengesa ise kuoneka olakwa mumenso ya Farao na banchito bake. Iwe waika mukondo mumanja mwao kuti bati paye ise." ²² Mose anabwelela kuli Yehova naku kamba kuti, "Ambuye, nichani mwanitumila ine kuno?" ²³ Kuchokela pamene nin bwelela kuli Farao kukamba kuli enve muzina yanu, apangisa mabvuto kuli bantu aba, anso simunaleke bantu banu kumasuka."

Chapter 6

¹ Yehova ankamba kuli Mose kuti, "Maje iwe uzaona vamene niza chita kuli Farao. Uzaona ichi, azabasiya kuti bayende chifukwa chakwanja yanga ya mpamvu, azabapisha benve mu ziko yake. ² Mulungu anakamba na Mose naku mu'za enve kuti, "Ine ndine Yehova. ³ Nina onekela kuli Abrahamu, kuli Isaki, na kuli Yakobo ngati Mulungu wa mpamvu zonse, koma na zina yanga, Yehova, sinenze ozibika kuli benve. ⁴ Ninapanga chipangano na benve, kuti abapase benve ziko mu kanani, muziko mwamene bana nkala monga sibene, mu ziko yamene banali kuzungulukamo. ⁵ Koma, nanvela kulila kwama isilayelu bamene a'Iguputo bapanga ukapolo, nakukubmukila chipangano changa. ⁶ Chifukwa chake, uzani ma Isilayeli, 'Ine ndine Yehova. Niza kakuchosani mu kapolo kuli bamu Iguputo, naku mumasulani imwe ku mpamvu ya chiweruzo. ⁷ Niza kamutangani imwe ngati bantu banga, ine nizakankala Mulungu wanu. Muzakazibika kuti ine nfine Yehova Mulungu wanu, wamene ana kuchosani imwe mu ukapolo wa Iguputo. ⁸ Niza kubwezani imwe ku ziko yamene nina lumbila kuti nizapasa Abrahamu, na kuli Isaki, na kuli Yakobo. Niza kupasni imwe kunkala chintu chanu. Ine ndine Yehova." ⁹ Pamene Mose anauza ivi kuli ma Isilayeli, sibana munvelele chifukwa chokumusiwa na ukali wa ukapolo. ¹⁰ Pamene apo Yehova anakamba kuli Mose, kuti, ¹¹ "Yenda uka Farao, mfumu wa Iguputo, kuti aleke bantu bamu Isilayeli kuchoka pa malo yake." ¹² Mose ankamba kuli Yehova, "Ngati ma Isilayeli sibana ninvelele ine, nichani Farao azani nvelele ine, kupeza sinikamba bwino?" ¹³ Yehova anakamba kuli Mose na Aroni. Anaba pasa lamulo ya Isilayeli na Farao, mfumu ya Iguputo, kuchosa ma Isilayeli mu ziko ya Iguputo. ¹⁴ Aba ndiye benze basogoleli bama nyumba yaba tate babo: Bana bamuna ba Rubeni, oyamba kubadwa kuli Isilayeli, benze Hanoki, Pallu, Hezron, na Karmi. Banali makolo ba banja ya Rubeni. ¹⁵ Bana bamuna ba Simion banali Jemueli, Jamini, Ohad, Jakin, Zohar, na Shaul-mwana mwamuna wa mukazi wamu kanani. Banali makolo ba banja ya Simion. ¹⁶ Aya ndiye ma zina yanali yo lembewaya bana bamuna ba Levi, pamozi na mibadwo yabo. Banali Gershon, Kohath, na Merari. levi anankala mpaka zaka 137. ¹⁷ Bana bamuna ba Gershoni banali Libni na Shimei, muma banja yabo. ¹⁸ Bana bamuna ba Kohath banali Amram, Izar, Hebroni na Uzziel. Kohath anankala zaka 133. ¹⁹ Bana bamuna ba Meriri banali Mahli na Mushi. Aba banankala makolo ya banja yama Levi, pamozi namubadwo yabo. ²⁰ Amram anakwatila Jochebed, mulongosi wa batate bake. Anamubalila Aroni an Mose. Amram anankala zaka 137 nakufa. ²¹ Bana bamuna Izar banali Kora, Nefegi, na Zichri. ²² Bana bamuna ba Uzziel banali Mishael, Elzafani, na Sithri. ²³ Aroni anakwatila Elisheba, mwana mukazi wa Amminadab, mulongozi wa Nahshon. Enve anamubalila Nadab na Abihu, Eleazar na Ithamar. ²⁴ Bana bamuna ba Kora banali Assir, Elkana, na Abiasaf. Bana nkala makolo ya banja ya Korahites. ²⁵ Eleazar, mwana mwamuna wa Aroni, anakwatila umozi mwana mukazi wa Putiel. Nakumubalila Phinehas. Aba banali basogoleli bama nyumba na ma banja yawo. ²⁶ Aba bamuna ba bili banali Aroni na Mose bamene Yehova anauza kuti, "Chosani ma Isilayeli mu ziko ya Iguputo nama gulu ya amuna ba nkondo." ²⁷ Aroni na Mose bankamba na Farao, mfumu wa Iguputo, vomelesa kuchosa ba Isilayeli ku Iguputo. Aba banali ba mozi Mose na Aroni. ^{28 29 30} Pamene Yehova anakamba na Mose mu ziko ya Iguputo, Enve anakamba kuli enve, "Ine ndine Yehova. Kamba kuli Farao, mfumu wa Iguputo, vonse vamene niza ku'za." koma Mose anakamba kuli Yehova, "Siniziba kukamba bwino, nichani chamene Farao zani nvelele ine?"

Chapter 7

¹ Jehova anakamba kuli Mose kuti, "Ona, Nakupanga monga mulungu kuli Farao. Aroni mubale wako azankala mneneri wako. ² Iwe uzakamba vonse vamene nizaku lamulila, Aroni mubale wako ndiye azakamba na Faaro kuti aba lake bana ba Isireli ba chokemo mu malo yake. ³ Koma niza mulimbisa mutima Farao, kuchoka apo niza langiza vounesa mpamvu zanga, zambiri zodabwisa, mu malo ya Egpto. ⁴ Koma Farao saza munvererani, kuchoka apo nizaika kwanja yanga pa Egpto naku chosa ma gulu yanga ya amuna omenyana, bantu banga, bantu baku Isireli, choka ku a,lo ya Egpto na vilango. ⁵ Egpto izaziba ati ndine Yehova nikafikiza kwanja yanga pa malo ya Egpto naku chossa ma Isireli pakati pao. ⁶ Mose na Aroni anachita sochabe; banachita monga mwamene Yehova analamulila. ⁷ Mose anali na zaka ayite, na Aroni anali na zaka ayite fili pamene bana kamba na Farao. ⁸ Yehova anakamba kuli Mose na kuli Aroni, ⁹ Pamene Farao azakamba kuli imwe `chitankoni cho dabwisana,' kuchoka apo uza kamba kuli Aroni, `Tenga nkoli yako uyi ponye pansu pal Farao, kuti isanduke njoka. ¹⁰ Mose na Aroni banayendakuli Farao, naku chita vamene Yehova analamulila. Aroni anaponya pali Farao na nchito bake, naku bwela ku nkala njoka. ¹¹ Pamene apo Farao anayitana ba nzeru na ng'anga zake. banachita monga majik yabo. ¹² Mwamuna aliyense anaponya nkoli yake, chokonkapo nkoli inankala njoka. kom nkoli ay Aroni inamela njoka zabo. ¹³ Mutima wa Farao wenze unakosesewa anso sananvele, monga Yehova anakambila. ¹⁴ Yehova anakamba kuli Mose kuti, "Mutima wa Farao ni olimba, kuchoka apo anakana kubaleka bantu bayende. ¹⁵ Mukayende kuli Farao kuseni pamene azayenda ku manzi. muka imilile ku mbali kwa manzi muka mukumane, ndipo uka nyamule mumanja mwako nkoli yamene yenze ina sanduka njoka. ¹⁶ Mu'uze kuti, `Yehova, Mulungu wa Ahebri, anitumma kuli iwe kukamba kuti, "Leka bantu banga bayende, chakuti baka niymike muchipulu. Namanje sumunanvele." ¹⁷ Yehova akamba kuti: chifukwa chaivi muzaziba kuti ndine Yehova. niza pana manzi yaka mumana ka Nile na nkoli ya kwanja yanga, kuchoka apo ka mumana kazankala magari. ¹⁸ Nsomba zili muka mumana zizafa, naka mumana kazanunka. Ma Egpto sibaza nkwansia kumwa manzi yamu ka mumana. ¹⁹ kuchoka apo Yehova anauza Mose, "mu.uze Aroni," Tenga nkoli utambulule kwanja yako pa manzi ya Egpto, na pali kamumana, kamumana, ponkala manzi, na mosungila nsomba, kuti manzi yabo yankala magari. chitanso kuti munkale magari pa malo ya Egpto, namu vu gubu va planga na myala. ²⁰ Mose na Aroni banachita vamene anabalamulila munlungu. Aroni ananyamula nkoli naku menya pa manzi yamu ka mumana, pamenso ya Farao naba nchito bake. Mumana onse unasanduka magari. ²¹ Nsomba inali muka mumana infa naka mumana kanayamba kununka. Ma Egpto sibana kwanise kumwa manzi yamu musanje na magari yenzeli pa malo ya Egpto. ²² Koma ba majik baku Egpto banachita monga benve na majik yabo. chokonkapo mutima wa Farao unalimba, nakukana nvelella Mose na Aroni, monga Yehova anakambila viza chitikila. ²³ Kuchoka apo Farao anakoneka noyenda munyumba mwaka. sanafakeko na nzelu. ²⁴ Ma Egpto bonse banakumba kumbali kwa kamumuna kuti bapeze manzi yokumwa, koma sibana kwanise kumwa manzi yamu kamunmana. ²⁵ Masiku yali seveni yanapita kuchokela pamene anapandila pa manzi

Chapter 8

¹ Pamene apo Yehova anakamba kuli Moe kuti, "Yenda kuli Farao naku mu'uzza enve, 'Yehova akamba ivi: "Leka bantu banga bayende kuti bakani pempeze in. ² Uka kana kubaleka kuyenda, niza vutisa ziko yako yonse nama chule. ³ Na kamumana kaza zul nama chule. Viza bwela pamwamba naku zula na kuyenda mu nyumba yako, kuchipinda kwako, napa bedi pako. Viza yenda muma nyumba ya banchito bako. Viza yenda kubantu bako, mumauveni yako, na namo sakani zila mwako. ⁴ Na machule yaza kumenya iwe, bantu bako, na banchito bako bonse."" ⁵ Yehova anakamba kuli Mose, "Mu'uze Aroni, "Tambulula kwanja yako na nkoli pali nyanja, tumumana, mwamene manzi nkalila, na ku bwelesa ma chule mu malo ya Iguputo." ⁶ Aroni ana anatambulula kwanja yake pamanzi ya Iguputo, naku ma chule yabwela pamwamba pa naku zula pa malo ya Iguputo. ⁷ Koma ba majiki bao bana bana chita mwamene banachitila na majiki yabo; bana bwelesa ma chule mumalo ya Iguputo. ⁸ Pamene Farao anaitana Mose na Aroni naku bauza, "Pmempelani kuli Yehova kuti enve achose ma chule pali ine na bantu banga. Ndiye pamene zibaleka bantu bayende kuti benve ba peleke nsembe kuli enve." ⁹ Mose anakamba kuli Farao, "Unga nkale namupata oniuza ine pamene ninga kupempelela iwe, banchito bako, na bantu bako, kuti ma chule bachosewe kuli iwe na muma nyumba na kunkala chabe mu mumana." ¹⁰ Farao anati, "mailo." Mose anati, "chinkale mwamene wa kambila, kuti uzibe iwe ati kulibe wina monga Yehova, Mulungu watu. ¹¹ Ma chule bazachoka kuli iwe, muma nyumba yako, banchito bako, na bantu bako. bazankala chabe mu mumana." ¹² Mose na Aroni banachoka pali Farao. Pamene apo Mose analila kuli Yehova pali vima chule vamene anabwelesa kuli Farao. ¹³ Yehova anachita monga Mose ana pempa: Ma chule banafela muma nyumba, makoti, na muminda. ¹⁴ Bantu banakolonganika pamozi, malo yaja yanali kununka. ¹⁵ Koma Pamene Farao anaona kuti amasuka, enve analimbisa mutima ndipo sana mvelele Mose na Aroni, monga mwamene Yehova anaba vamene azachita. ¹⁶ Yehova anakamba kuli Mose kuti, "Mu'uze Aroni, "Tambulula kwanja yako naku menya kalukungu kali pansi, kuti inkale natu doyo pa malo ya Iguputo." ¹⁷ Bana chita sochabe. Ndiye pamene Aroni anatambulula kwanja yake na nkoli pansi pa doti. Tudoyo tona bwela pa bantu na vi nyama. Yonse kalukungu inankala natu doyo pa malo yonse ya Iguputo. ¹⁸ Ba majik bana yesa majik yabo kuti ba pange tudoyo, koma ina kanga. Chakuti kunali tudoyo mu bantu na nama. ¹⁹ Pamene ba majik banakamba kuli Farao, "Ichi nichu kumo cha Mulungu." Koma Farao anakosesa mutima wake, na kukana kuba mvelela. Chinali mwamene Yehova anakamba Farao azachita. ²⁰ Yehova anakamba kuli Mose, "Nyamukani kuseni maningi na kuyenda kuimilila kuntangu ya Farao pamene akalibe kuyenda ku mumana. Mumu uze enve, "Yehova akamba ivi: "Basiye bantu banga bayende kuti bakani pempelele ine. ²¹ Ngati isuzza baleka bantu banga kuyenda, ine inza tuma gulu yaba inzi kuli iwe, banchito vbao, na bantu bako, na muma nyumba yabo. Manyumba yaba Iguputo yazankala nama gulu ya inzi, ndipo na pansi pamene badyaka paza nkala ba inzi bambili. ²² Koma siku ija ine mwamene niza tengela malo ya Gosheni, mosiyanako mumalo mwamene bantu banga bankala, chakuti gulu yaba inzi si'iza nkalako. Ivi vizachtika kuti ndine Yehova ali mumalo yanu. ²³ Ine niza faka chosiyanisa pali bantu banga na bantu bako. Cholangiza mpavu zanga chiza oneka mailo. ²⁴ Yehova ana chita so chabe, na gulu ikulu yama inzi ina bwela munyumba ya Farao na munyumba yaba nchito bake. Yonse malo ya Iguputo, malo yana onogeka chifukwa cha gulu yama inzi. ²⁵ Farao anaitana Mose na Aroni na kukamba kuti, "Yenda, Peleka nsembe mumalo yatu." ²⁶ Mose anakamba kuti, "Sichabwino ise kuchita ivo, chifukwa nsembe zamene tima peleka kuli Yehova Mulungu watu nizo nyansa kuli ba Iguputo. Ngati tapeleka nsembe bwino bwino mumenso yabo yo nyansa kuli ba Iguputo, sibaza titema myala? ²⁷ Iyai, nimasiku yatatu yo yenda muchipululu yamene tifunika kupanga, kuti tipeleke nsembe kuli Yehova Mulungu watu, mwamene anatilamulila. ²⁸ Farao anakamba, "ine niza kusiyani muyende ndipo mupeleke nsembe kuli Yehova Mulungu wanu muchipululu. Ngati simuza yenda kutali. nipempeleleni ine." ²⁹ Mose anakamba, "nika choka chabe pano, niza ma inzi yaku kuli Yehova kuti ma gulu yama inzi yaku siye, Farao, Banchito bako na bantu mailo. Koma usa chitenso boza paku salekelela bantu batu kupeleka nsembe kuli Yehova." ³⁰ Mose ana choka pali Farao na kuyenda kupempela kuli Yehova. ³¹ Yehova anachita vamene Mose anapempela; na kuchosa magulu yaba inzi kuli Farao, banchito bake, pa bantu bake. kulibe nangu kamozi kanasala. ³² Koma pantawi iyi Farao ana limbisa mutima wake. ndipo sana baleke bantu kuyenda.

Chapter 9

¹ Pamene Yehova anakamba kuli Mose, "Yenda kuli Farao na kumu uza, 'Yehova, Mulungu wa Aheberi, akamba ivi: "Leka bantu banga bayende kuti bakani pempeze." ² Koma ngati iwe wakana kubaleka bayende, ngati wapitiliza kuba sungilila, ³ pamene kwanja ya Yehova iza leta vili mu munda-hachi, ma bulu,ngamila, ng'ombe na mbelele. ⁴ Koma Yehova azaka panga kusiyanisa pakati pa vobeta vaku Isilayeli na vobeta vaku Iguputo, kuti kusankale nyama yaba Isilayeli isakafa. ⁵ Yehova akonza ntawi; akamba kuti, "mailo pamene nizakachita ivi vintu mu malo." ⁶ Yehova anachita ivi siku yo konkapo: vonse ng'ombe zaku Iguputo zinafa, koma kulibe nyama zaba Isilayeli zinafa, kulibe olo imozi. ⁷ Farao ana funsa funsa, na, onanoni, kunalibe nangu nyama imozi yaba Isilayeli inafa. Koma mutima wake unali oyuma, mwaicho sanaba leke bantu kuti bayende. ⁸ Pamene Yehova anakamba kuli Mose nakuli Aroni, "Tengakoni milota mu oveni kuzuzya kwanja. Iwe, Mose, ufunika kuponya milota mu mpepmo ninshi Farao atamba. ⁹ Viza nkala lukungu yopepuka pa malo ya Iguputo. Viza lengesa vituza na vilonda ku choka ku bantu na ku nyama mu malo yonse ya Iguputo." ¹⁰ Pamene apo Mose na Aroni banatenga milota mu oveni naku imilila pa sogolo pa Farao. Pamene apo Mose anaponya milota mumpopo. Milota zina lengesa vituzi na vilonda ku chika mu bantu na vinyama. ¹¹ Bana Yele bana kangiwa kumu lesa Mose chifukwa chavituza, chifukwa vituza banali navituza na bonse bama yele benangu. ¹² Yehova analimbisa mutima wa Farao, chakuti Farao sana mvelele Mose na Aroni. Ivi vinali monga anakambila kuli Mose mwamene Farao azachitila. ¹³ Pamene apo Yehova anakamba kuli Mose kuti, "Uka uke kuseni seni, uka imilile pa sogolo pa Farao na kukamba kuli enve, 'Yehova, Mulungu wa Aheberi, akamba ivi: :Leka bantu banga ba yende kuti bakani pempeze. ¹⁴ Chifukwa ino ntawi nizatuma vonse vilango vanga pali imwe, pali banchito banu na bantu banu. Niza chita ini kuti ungazibe kuti kulibe muntu monga ine mu ziko yonse yapansi. ¹⁵ Pali manje sembe na tambasula kudala kwanja nakuku ukila nama tenda iwe na bantu bako ngati mwa chose wapo pa malo. ¹⁶ Koma nichifukwa cha ichi ninaku vomelekezani kuti mupulumuke: kuti niku langizeni imwe mpamvu zanga, chakuti zina yanga ikambiwe ziko yonse ya pansi. ¹⁷ Ukali uzinyamula pa bantu banga naku kana kubaleka bayende. ¹⁸ Mvelani! Mailo ntawi mnga yamene iyi nizakaleta chi mpepo cha mpamvu chamene cikalibe kuonekapo mu Iguputo kuchokela pa siku inayamba mpaka lelo. ¹⁹ Apa manje, tuma namuna baike pamozi vibeta vanu na vonse muli navo mu mininda ku malo yo tetezewa. Aliyense muntu na nyama zamene zili mu munda ndipo sizina bwele kunyumba mu mund-matala yaza vigwela, ndipo vizafa. ²⁰ Pamene banchitio ba Farao bana kulupilila mu utenga wa Yehova. bana yendesa naku ileta bakapolo babo na vibeto vabo mu manyumba. ²¹ Koma baja bamene sibana tenge utenga wa Yehova ma fakilako nzelu bana siya ba kapolo babo na vibeto vabo mu minda. ²² Pamene Yehova anakamba kuli Mose, "Nyamula kwanja yako mu mwamba kuti kunkali ngozi monse mumalo ya Iguputo." Pa bantu na vinyama, napa vonse vomela mu minda mu malo ya Iguputo." ²³ Mose ananyamula nkoli yake mu mulenga lenga, ndipo Yehova anatuma chimpepo chikulu, matalala na kaleza pansi. Analokesa mwa ngozi pa malo Iguputo. ²⁴ Chakuti kunaki malata yo sankaniza na tuleza, yakali maningi, yamene yakalibe kuchitikapo monse mu malo ya Iguputo kuchokela pamene inankalila ziko. ²⁵ Monse mumalo ya Iguputo, matalala yana gwela vonse vinali mu minda bantu pamozi navi nyama. Vina gwela pa vomela vonse vamu minfa naku tyola mitengo zonse. ²⁶ Koma kumalo ya Gosheni, kwane kunali kunkala ba Isilayeli kunalibe matalala. ²⁷ Pamene apo Farao anatuma bantu kuti baitane Mose na Aroni. Anakamba kulibenve, Ine nachimwa ino ntawi, ehova nii olungama, na ine na bantu banga ndise boipa. ²⁸ Pempelani kuli Yehova chifukwa tuleza tukulu na malata ya pakisa maningi. nizakulekani muyende, ndipo simuzankala pano." ²⁹ Mose anakamba kuli enve, "Pamene apja chabe nikachokamo mu muzinda, niza vungulula mana yanga kuli Yehova. Tuleza tuzasiya, ndipo sikuzankala futi malata. Munjila iyi muza ziba kuti ziko yapansi niya Yehova. ³⁰ Koma kwa imwe naba ncito banu, Ine niziba kuti simu lemekeza Yehova Mulungu." ³¹ Manje tonje na belele vina onogeka, chifukwa belele inali yokula pachimate mu matu na tonje inali kuchosa maluba. ³² Koma tirigu na rai sivina onongeke. chifukwa vinali voshanga ntawi yaku sogolo. ³³ Pamene Mose anasiya Farao na muzinda, anavumbulula manja yake kuli Yehova; tuleza na malata vina leka. na mvula ina leka kugwa. ³⁴ Pamene Farao anaona kuti mvula, malata na tuleza va leka, anachimwa futi naku limbisa mutima wake, pamozi na banchiti bake. ³⁵ Mutima wa Farao unankala olimba, chakuti sanaba leke bantu kuyenda, monga mwamene Yehova anakambila mu kwanja ya Mose.

Chapter 10

¹ Yehova anakamba Kuli Mose Kuti, "Yenda kuli Farao, chifukwa na limbisa mutima wake na mutima zaba nchito bake. Ine nachita ivi kuti nilangize mpavu zanga pakati pawo. ² Ine nachita ivi kuti muka buaze bana banu na bazukulu vintu vamene nachita, nayi sunga kuipa Egpto, anso na pasa zizindikilo zosiyana kulangiza mpamvu yanga pakati pawo. mwaso muzaziba ati ine ndine Yehova" ³ Kuchoka apo Mose na Aroni banayenda kuli Farao naku mu'uzi Yehova, Mulungu wa Aheberi, akamba ivi: muzakana kufika liti kuzichepesa pamaso panga? Leka bantu banga bayende kuti bakaniyamike. ⁴ Koma ukakana kuba leka bantu banga kuyenda, nvela, mailo nizaleta vidiza pa malo yanu. ⁵ Viza vininkila pa mwamba pa malo kuti kulibe azayamba kuona pa ziko ya pansi. Bazadya vamene viza salako vina taba mu matalala. Vizadya mitengo yamene ikula mu munda. ⁶ Viza zula muma nyumba yanu, nayaba nchito banu, na binse bamu Egpto - chamene batate bako olo ba mbuya bako bakalibe kuonapo, kulibe kuchokela pamene bana nkala pa ziko ya pansi kufika siku ya lelo. kuchoka apo Mose anachokapo pali Farao noyenda. ⁷ Banachito ba Farao banamu'uzi, "Uyu mwamuna azaleka kuti vutisa liti? Leka bayende baku Isireli kuti baka nimpempeze Yehova Mulungu wabo. ninshi simuona ati Egpto ya onongeka?" ⁸ Mose na Aroni banaleta futi kuli Farao, anakamba kuli benve," yendani kuli Yehova Mulungu wanu muka mu pempeze. Koma nibati bantu bazayenda?" ⁹ Mose anakamba, "Tiza yenda naba ngono batu naba kulu batu, bana batu bamuna na bakazi. Tienda na gulu ya vobeta na ng'ombe yatu, chifukwa tizankala nama dyelelo ya Yehova. ¹⁰ Farao anabauza, Yehova ankale naimwe, nikaku lekani muyende natu ngo'no twanu kuyenda. Onani, mulina voipa mu nzeli zanu. ¹¹ Iyayi! yenda, bamuna beka pakati pako, naku mpepeza Yehov, kaili ndiye vamene mufuna." Kuchoka apo Mose na Aroni bana ba pisha pamaso ya Farao. ¹² ¹³ Yehova anakamba kuli Mose, "Tambulula kwanja yako pa malo ya Egpto kuli vidiza, kuti vika menye malo ya Egpto na kudya vomela vilimo, vonse matalala yana sala." Mose ana tambulula nkoli yake pa malo ya Egpto, chokonkapo Yehova analeta chimpepo chaku mawa pa malo yaku Egpto muzuba monse na usiku. Pamene kunali kuseni, chimpepo chaku mawa chinaleta vidiza ¹⁴ Madiza yana yenda pa malo yonse ya Egpto naku zula konse, pakalibe kuonekako chikalile ku nyinji wa mutundunuyu wa madiza, kulibe yopalana ivi vizaka bwelapo nafuti. ¹⁵ Vina vininkila pa mwamba pa malo ya Egpto kuti kunankala na mudima. Vinadya vomela na vonse vi vipaso vaku mitengo yamene matalala yana siya. Pa malo yonse Egpto, palibe chamoyo chomela chinasala, olo mitengo na chomela mu munda. ¹⁶ Pamene Farao anayitana mwamusanga Mose na Aroni naku kamba, "Nachimwa kuli Yehova Mulungu wanu naimwe. ¹⁷ Anso pano, nikululukileni ma chimo yanga pa ntawi ino, anso mupempele kuli Yehova Mulungu wanu achose infa pali une." ¹⁸ kuchoka apo Mose anachokapo pali Farao naku pempela kuli Yehova. ¹⁹ Yehova analeta chi mpepo cha mpamvu kumazulo nonyamula vi iza novi peleka mukamumana yama tete; sipanasale vidiza vili vons pa malile ya Egpto. ²⁰ Koma mulungu ana limbisa mutima wa Farao, anso Farao sanabaleke ba Isireli kuyenda. ²¹ Kuchoka apo Yehova anakamba kuli Mose kuti, "Tambulula manja yako ku mwamba, kuti ku nkale mudima pa malo ya Egpto, mudima wa bii." ²² Mose anatambulula manja yake ku mwamba, ndipo kunali mudima bii mu malo ya Egpto masiku yatatu. ²³ Palibe anali kuona aliyense; palibe anachoka pa nyumba pake masiku yatatu. mwaicho, kunali nkunkala ma Isireli kunali kotuba. ²⁴ Farao anaitana Mose naku kamba kuti. "Yenda uka mu pempeze Yehova. nama banja yanu yanga yende naiwe, koma gulu ya vobeta na ng'ombe mu siye." ²⁵ Koma Mose anakamba kuti, "Tivomelesenu tinkale navo peleka vo shoka kuli Yehova Mulungu watu. ²⁶ Ng'ombe zatu zifunika kuyenda naise; kulibe bologodoili yonse izasala kumbuyo, chifykwa tizafunika kuti tika pempeza Yehova Mulungu watu chifukwa sitiziba vamene vo pempelezako Yehova mpaka tikafika kuja." ²⁷ Koma Yehova anakosesa mutima wa Farao, anso sanaba lekelele kuyenda. ²⁸ Farao anati kuli Mose, "choka pali ine! samalani pali chintu chimozi, kuti musaka ni onepo futi, chifukwa siku muzaka ana nfeshi yanga, muzakafa." ²⁹ Mose anakamba kuti, "Iwe weka wakamba sinizaka onapo nfeshi yaku nafuti."

Chapter 11

¹ Pamene Yehova anakamba kuli Mose, "kuliko umozi mulili wamene nizabwelesa kuli Farao na Iguputo. Pambuyo pake, azakuvomelesani kuti muchokemo muno. ² Pamene azakuvomelesani kuyenda, azakuchosani. Bauze bantu kuti mwamunaa na mukazi aliyense afunika kupempa kuli munzake wapafupi vabwino ba siliva na golide." ³ Manje Yehova analengesa A'iguputo kuti bakondelese bana ba Isilayeli. Pamwamba pake, mwamuna Mose anali ukondwelesewa pa menso ya ba nchito ba Farao na bantu ba mu Iguputo. ⁴ Mose anakamba kuti, "Yehova akamba ivi: 'Pakati pa usiku nizayenda monse mu Iguputo. ⁵ Bonse bana boyamba muziko ya Iguputo bazafa kuyambila mwana uyamba wa Farao wa Farao, wamene ankala pa mupando ya mfumu, kufikila mwana oyamba wa mukazi wamene ankala pa myala ypoela, na bana bonse ba ba vobeta vabo. ⁶ Pamene kuzankala kulila mu ziko yonse ya Iguputo, mwamene sikunakalepo olo sikuzankalapo futi. ⁷ Koma palibe nangu galu azauwapo pa bana ba Isilayeli, ngankale pa muntu kapena chinyama mwaichi. ⁸ Aba bonse banchito bako, Farao, bazabwela kuli ine na kunigwadila ine. Bazakmba, yenda, iwena bantu bonse bamene ba kukonka pambuyo pa izo niza chokapo; Pamene apo anachoka pali Farao mu ukali kwambili. ^{9 10} Yehova anakamba kuli Mose kuti, "Farao sazaku nvelela. Nichifukwa niza chita vintu vodabwisa vambili mu ziko ya Iguputo. MOse na Aroni banachita vonse ivi vodabwisa pamenso ya Farao. Koma Mulungu anakosesa mutima wa Farao, anso Farao sana vomekeze bantu ba Isilayeli kutuluka mu malo mwake.

Chapter 12

¹ Mose anaika pamozi gulu ya bana ba Isilayeli naku bauza kuti, "Ivi ndiye vintu vamene Yehova analamulila kuchita. ² Pa masiku sikisi nchito ingagwililewe, koma kuli imwe, siku ya seveni ifunika kunkala yoyela, siku ya Sabata niyopumulatu, yoyela kuli Yehova. Aliyense wamene agwila nchito iliyonse pa siku iyo afunikila kupaiwa. ³ Simufunikila kuyasha mulilo munyumba iliyonse pamsiku ya Sabata." ⁴ Mose anakamba na gulu ya Isi, kukamba kuti, "Ichi ndiye chintu chamene Yehova alamulila. ⁵ Mupeleke pelekelo kuli Yehova, bonse ba imwe muli na mutima ofunisa. Muletee chopeleka kuli Yehova.-golide, siliva, mukwa, ⁶ bulu, pepo, na tonje na nyula yopepuka; masako ya mbuzi; ⁷ chikumba cha mbelele chamaonekedwe ya daya ya redi; ⁸ mafuta ya mnyala ya malo yopatulika, vonunkilisa mafuta yozozela na chifungo yabwino, ⁹ myala ya onika na myala zinangu zabwino kuti vi'ikiwe pa efodi napa nyula ya pachifuba. ¹⁰ Mwamuna aliyense wa uiso pakati pa imwe abwele na kupanga vilivonse vamene Yehova alamulila- ¹¹ kachisi na chihema zake, chovininkila, chofyantila cake, mafelelmu, togwililila, sandamile, na maizko; ¹² futi likasa na sandamika zake, chovininkila cha chitetezo, na nyula yachobisila. ¹³ Banaleta tebo na nsandamila zake, na mukate wa pamenso pa mulungu; ¹⁴ na choikap nyale, yo sanikila na vosebenzela vake, nyale zake, na mafuta ya munyale; ¹⁵ Vonunkila yapaguwa na nsandamila zake, mafuta yozezelewa na fungo yabwino: chinyula chovalila pa chiseko; ¹⁶ guwa yoshokelapo vopeleka na kabati ya mukuwa na nsandamila zake na vosebenzela; na dishi ikulu maziko yake. ¹⁷ Banaleta volelenga va pamalo ya panja na nsandamila zake na maziko, na kelani ya panja pongenela; ¹⁸ na chopinila cha chihema cha kachisi na panja pamozi na ntambo zake. ¹⁹ Banaleta mukanjo yopepuka yotungiwa bwino yosebenzesa mu malo yoyela, mikanjo yoyela ya Aroni wansembe na bana bake bamuna kuti batumikike ngati bansembe. ²⁰ Pamene apo gulu yonsr ya bana ba Isilaeli banachokapo pamenso pa Mose. ²¹ Aliyense wamene mutima wake unagwidwa wamene muzimu wake unapanga kufunisisa anabwela na nakuleta chopeleka kuli Yehova kuti bapangile kachisi, vonse vintu vautumiki mukati, na mikanjo zoyela. ²² Banabwela, bonse bamuna na bakazi, bonse benze na mutima ofunisisa. Banaleta tubangili, mpete za kumatu, za kukakumo, na vokonngoles na mutundu yonsr ya jeweli ya golide. Bonse banaleta chopeleka cha golide kuli Yehova munga chopeleka cha chonesela. ²³ Aliyense enzeli na bulu, pepo, kapena tonje yofila, nyula yopepuka, chikumba cha mbuzi chikumba cha mbelele cha maonekedwe ya redi, kapena chikumba chopepuka vinaletawa kuli benve. ²⁴ Aliyense opanga chopeleka cha siliva kapena mukwa banaleta munga chopeleka kuli Yehova, ndipo aliyense wamene anali na mutengo wa akesha ku'ugwilisila nchito iliyonse banaleta. ²⁵ Aliyense mukazi wa luso yotunga tonje na manja yake, analeta vamene banatunga bulu, pepo kapena tonje yofila, kapena nyula yopepuka. ²⁶ Bakazi bonse bamene mutima wabo unfunisisa na benzeli na luso yopana masako yambuzi. ²⁷ Basogoleli banaleta myala ya oniki na myala yobeka kuti yaikiwe pa efodi na chachifuba; ²⁸ Banaleta vonunkisa na mafuta ya munyale, va mafuta yozozelako naya fungo yabwino. ²⁹ Ba Isilayeli banaleta chopeleka mosakakamiziwa kuli yehova mwamuna na mukazi aliyense wamene mutima wake unafuna analeta vintu va nchito yonse yamene Yehova analamulila kupitila muli Mose kuti chipangiwe. ³⁰ Mose anakamba kuli ba Isilayeli, "onani, Yehova aitana pa zina pa Bazale, mwana mwamuna wa Uri mwana mwamuna wa Huri, kuchokela ku mutundu wa Yuda. ³¹ Anazulisa Bazala na muzimu wake, kumupasa nzelu, kumvesesa, naku ziba, kuli mutundu yonse yopanga za manje, ³² kupanga zaluso na kusebenza mu golide, siliva, na mukwa; ³³ futi ku juba na kuika myala na kusema mitengo-kuchita mutundu yonse ya luso na kupanga va manja. ³⁴ Wachika mu mutima mwake kuchipunzisa, bonse benze na Oholiabu mwana mwamuna wa Ahisamaki, kuchokela mu mutundu wa Dani. ³⁵ Wabazuzya na luso kuchita mutundu yonse ya nchito, ku sebenza munga opanga, bokumba, botunga mu bulu, pepo na vofila na nyula yopepuka, ndipo munga mukanjo. Nibaluso mu nchito zosiyana siyana, na bopanga.

Chapter 36

¹ Chakuti Bazalo na Oholiabi naba kaswili bamene Yehova anapasa paso mpamvu zoziba kuchta nchio yomanga malo yoyela nachito zamene Yehova anaba lamulila." ² MOse anaitana Bazalo, Oholiab, na bonse bakaswili bamene Yehova anafasa paso, na uli onse wamene mutima wake unanyamulisa kuchita nchito. ³ Banalandila kuchokela kuli Mose chopeleka chamene ba Isilayeli bana leta kumangila malo yoyela. Bantu benze bakali kuleta vopeleka kuli MOse pamutima wawo siku zonse. ⁴ Chakuti bakaswili bonse banalikusebenza pa malo yoyela bana sebenza kuli vamene banali kuchita. ⁵ Bobaza banuza Mose. "Bantu baletavambili kuli vamene vifunika kuchita nchito yamene Mulungu anatilamulia kuchita." ⁶ Chakuti Mose analesa bantu bamugulu kuleta vopeleka vomangila malo yoyela. Pamene apo bantu bana leka kuleta paso. ⁷ Banali navintu vambili vo chitila nchito. ⁸ Bonse bobaza pakati pawo banamanga malo yopempelelamo na nyula yolingana zili teni kuchokela kunyula ya tonje naya bulu, pepo, na nsalu ya maonekelo ya kelubi. Iyi inali nchito ya Bazlo, na bonse akaswili obaza. ⁹ Utali wa nyula iliyonse inali twenti-eyiti mikono, bufupi unali fo mikono. Nyula zonse zenze zo lingana. ¹⁰ Bazalo anakumanisa nyula zili faivi pamozi, na nyula zinangu zili faivi anakumanisa. ¹¹ Anapanga ntambo ya bulu mumbal msilisa nyula imozi, anachita vamene mwa nyula inakonkapo. ¹² Anapanga ntambo zili fifite pa nyula yoyambila na ntambo zili fifite mumbali mwanyula inakonkapo. Ntambo zinali zosiyana mumbali ina na mumbali ina. ¹³ Anapanga vogwilila va golide vili fifite nakuzi kumanisa pamozi nazina zachi kuti malo yopempelelamo yankale yogwili zana. ¹⁴ Bazalo anapanga nyula yachikumba chambuzi cha tenti yapa malo yopempelelamo; anapanga nyula izi zili leveni. ¹⁵ Utali wa nyula izi wnze sate mikono, na mufupi wa nyula yonse unali fo mikono. ¹⁶ Pa nyula zizli leveni zonse zanali zolingana. Anakumanisa nyula zili faivi pamozi na nula zili sikisi pamozi. ¹⁷ Anapanga ntambo zili fifite mumbali mwa nyula yoyambila, nantambo zili fifite mumbali mwanuyula nozikumanisa kuli zinakonkapo. ¹⁸ Bazalo anapanga vogwiliza va bronzi vili fifite kugwila tenti pamozi kuti inkale imozi. ¹⁹ Anapangila malo yo pempelelamo chivininkilo chinangu chachikumba chotelela chianli pamusamba. ²⁰ Bazalo anapanga mafulemu yoyimilia ya mutengo ya akesia yapa malo ya kachisi. ²¹ Utali wama fulemu unali mikono, na mufupi wafulemu ulionse unali mukono umozi napakati. ²² Fulemu ulionse inali nama pegisi yama pulanga yabili. Anachita vamene ivi kuma fulemu yonse yapa malo yopempelelamo. ²³ Anapanga mafulemu yamalo yopempelelamo munjila iyi: twenti fulemu kumbali yakumwela. ²⁴ Bazalo anapanga vapansi pamafulemu ya siliva zili fote zofaka pansi pafulemu kugwilisa mafulemu pamozi. ²⁵ Kumbali kwina kwa malo yopempelelamo, ku moto, anapanga mafulemu twenti. Nava pansi va siliva vili fote. ²⁶ Kunali vampansi vibili apsni pa fulemu yoyamba, vampansi vibili pali ina kukonkapo, no konkanya. ²⁷ Kumbuyo kwa malo yopempelelamo kumazulo, Bazalo anapanga ma fulemu sikisi. ²⁸ Anapanga ma fulemu yabili pa kona kumbuyo kwa malo yopempelelamo. ²⁹ Aya mafulemu siyenze yokatana pansi, kona yenze yokumana pamwamba na mpete. Anapanga yabili manjila iyi mumakona yabili. ³⁰ Yenzeli mafulemu eyiti, pamozi naza pansi za siliva. Zinali sikisitini zapansi pamozi, zapansi zibili pa fulemu yoyambila, zibili zapansi pa fulemu ina konkapo, nakupitilza. ³¹ Bazalo anapanga mutanda na mutengo wa akasiya-faivi mafulemu kumbali imozi yamalo yopempelelamo, ³² mitanda ili faivi yama fulemu kumbali jwina kwa malo yopempelelamo, na mitanda ili faivi kuma fulemu yakumbuyo kwa malo yopempelelamo ku mazulo. ³³ Anapanga mitanda pakati pama fulemu, ndiye pakati, kufika kosilila. ³⁴ Anapanga mafulemu na golide, anapanga mpete ya golide, kuti yakale chogwila chamitanda, anavalisa mitanda na goldie. ³⁵ Bazalo anapanga nyula za bulu, pepo na redi, nyula za tonje, yo'oneka monga kelubi, nchito ya kaswili. ³⁶ Anapanga nyula za nsandamila zili fo kuchokela kumutengo wa akasile, nakuzi valikapo golide. Anapanga nazo kobekela za golide muma nsandamila nakuzi ponyela pali zapansi za siliva zili fo. ³⁷ Anapanga chokobekela pongenela mu tenti. china pangiwa na bulu, pepo, redi na nyula ya tonje, nchito yabo tunga. ³⁸ Anapanga mokobekela mo pa nsandimila zili faivi na nkobekelo. Anazivalika pamwamba na nkoli na golide. zza pansi zili faivi zinali zo pangiwa na bronzi.

Chapter 37

¹ Bazalo anapanga likasa kuchokela ku mutengo wa akashiya. kotalimpa kwake kunali kokwanila mikono tu na hafu; mukufupikila kwake wanu na hafu mikono, na kotalimpa mikono wanu na hafu; ² Anavininkilamo mukati na kunja na golide yoyela nakuika mumbali mwake golide na pa mwamba pake. ³ Anaikapo mpete zinai za golide pasni pa mendo yak yinai, kumbali kumozzi, mpete zibili, na kumbali ina mpete zibili. ⁴ Anapanga sandamina ya mutengo ya akashiya na golide. ⁵ Anamikiza sandamina mukati mwa mpete ku mbali kwa sandamina, kuti itandizile kunyamula likasa. ⁶ Anapanga chotetezelako chovininkila cha golide yoyela. Kotalimpa kwake tu na hafu mikono na mukufupika kwake kunali wanu na hafu mikono yake. ⁷ Bazalo anapanga makelubi yabili kuchokelamku golide yomenyewa, kosiliza kubili kwa vininkila yotetezela. ⁸ Kelubi umozi onali kosiliza kwa vininkilo yotetezela. na kelubi wina anali kosiliza kwina. zinali zopanga ka mogwilizana na vininkilo yoteteza. ⁹ Na makelubi yana tambulula mapapiko yao kumwamba nakuchinga vininkilo yotete pakati pa vininkilo yotetezela. ¹⁰ Bazalo anapanga tebulo yochokela ku mutengo wa akashiya. kotalika kwake mikono ibili kufupika kwake mikono ili umodzi, nakutalika inali mikono umozi na hafu. ¹¹ Anavininkila na golide yosukwa bwino kuika mbali mwake na golide yosukiwa bwino. pamwamba pake. ¹² Anapanga chamumbali kukula kwake monga kwanja, na kuikako golide. ¹³ Anaikako mpete zinai za golide nauikapo mpete kumbali zonse zinai, kwamene muyendo inai inali. ¹⁴ Mpete inali yolumikiza ku chamumbali, kupeleka malo yonyamulila tebulu. ¹⁵ Anapanga sandamina kuchokela ku mutengo wa akashiya naku ivinnkila na golide, kuti akwanilise kunyamula tebulu. ¹⁶ Anapanaga vintu vamene vinali kufunikila pa tebulo, mbale, masipuni, mabeseni na nigomo kusebenzsea popoeleka vopeleka. Anapanga vonse kuchokela ku golide yosukiwa bwino nomenyewa. ¹⁷ Anapanga choikapo nyali kuchokela ku golide yosukiwa bwino yomenya. Anapanga choyikela nyali nachapansi chake na chapa mwamba chake. ¹⁸ Mbali mwake munlai mbanda zili sikisi - mbali iliyonse yoikapo nyali kunali zitatatu. mapnda yoyamba inali na makapu yatatu-monga maluba wopuka ya almondi, na chapansi chake na maluba, makapu yatatu monga maluba wopuka kumbali. ¹⁹ na chapansi chake na malubaq. chinali cholingana na vonse mpanda zili sikisi zo chokela ku choyikapo nyali. ²⁰ Pa choikapo nyali, chapakati, chake panali makapu yanai yopangiwa monga kupuka kwa almondi, na chapansi cha matepo na maluba. ²¹ Kunali chapansi, chamatepo pansi pa mpanda zibili zopangiwa monga chimozi, mwaizo chimozi mozi kunali chapansi chama tepo pansi pa chachitatu chazibili champanda, chopangiwa ngati chimozi, chinali chimozi mozi kuli vonse sikisi mpanda vochokela ku choikapo nyali. ²² Matepo ya pasni na mpanda zonse zinali chimozi. Mbali imozi inali yomonyee wa nchto ya golide yosuka bwino. ²³ Bazalo anapanga choyikapo nyalina nyali zili seveni, mbaniro na choyelapo pulusa cha golide youska bwino. ²⁴ Anapanga choyikapo nyali na zosebnzesa na gao imozi ya golide yoyela. ²⁵ Bazalo anapanga guwa yazonukila. Anapanga kusebenzesa mutengo wa akashiya. Kotalimpa kunali mukono umozi, na kufupika kwake mukono umozi. mbali zonse zinali zolingana na kotalumpa kwake kunali mukono ibili. Nsengo zake zinali zopangika ngati guwa imozi. ²⁶ Anavininkila guwa ya zonunikila na golide yosukiwa bwino pamwamba, mumbali na nsengo zake. Anapanganso na mbali mwake na golide. ²⁷ Anapanga mpete zibili za golide kuti igwile kosiliza kumbali zonse zubili zosiyanako. mpete zinali zogwililalna na pansi pa nsandamila yonyamulila likasa. ²⁸ Anapanga nsandamila ku mutengo wa akashiya. na kuyivinikila na golde. ²⁹ Anapanga mafuta yoyela yozozewekila kuti inukulishe bwino, nchito yaonukilisa.

Chapter 38

¹ Bazele anapanga guwa yoshekelapo nsembe ya mitengo. inali yolingana mu utali - na katatu kutalimpa kuyenda mu mwamba. ² Ana kulisako mumbali munali kuoneka monga nsengo za n'gombe. Nsengo zinali zogwilana na guwa, ndipo anavininkilapo na mkuwa. ³ Anapanga vonse vofunikoila va guwa - mpoto za milota, ma fosholo, madishi, vo pindamulilako nyama, na poika mulilo. Ndipo anapanga vonse vo funikila na mkuwa. ⁴ Anapanga komo ya guwa, mkuwa yo gwililila mitengo na poyakila mulilo. ⁵ Banapanga komo pansu pa limu inali kuzunguluka guwa. Bana ipanga mukati mwa guwa, panyansiko pan'gono kuti igwililile mitengo. ⁶ Bezele anapanga mizati yamitengo naku zivininkila na mkuwa. ⁷ Anaika mizati yamitengo mumbali mumbali mwa guwa, mo nyamulila. Anapanga guwa yamubo mukati kusebenzesa mapulnga. ⁸ Bezele anapanga choikilamo chikulu cham mkuwa. Anapanga choikilamo kusebenzesa magilasi ya bakazi bamene banali kusebenza pa komo ya hema yokumanilamo. ⁹ Anapanga chochingilizila hema kuzunguluka malo yokumanilamo. Nyula zakumbali kwa chochingilizila zinali zabwino, mukono handiledi kutalimpa. ¹⁰ Nyula zinali na poika pali twente, na mkuwa zili twente. Kunali to kobekelako moika, na ntambo za siliva. ¹¹ Chimozi naku malo ya ku mpoto, kunali vokobeka mikono handiledi kutalimpa na poika twente, na poika pa mkuwa pali twente, tokobekapo poikila, na nkoli za siliva. ¹² Vokobeka vaku mbali yaku mazulo zinali mikono fifite kutalimpa, na poika teni na vofakapo. Tokobekapo na ntambo zapoika zinali za siliva. ¹³ Chochingilizila chinali mikono fifite kutalimpa kumalo yakumwela. ¹⁴ Vokobeka kumbali imozi ya pongenela vinali mikono fifite kutalimpa. Vinali na poika patatu na vofakapo vitatu. ¹⁵ Kumalo kwina kongenela muchochingilizila kunali vokobeka va mikono fifite kutalimpa, Vinali na poika patatu na vofakapo vitatu. ¹⁶ Vonse vokobeka vinali kuzunguluka chochingilizila vinali vabwino. ¹⁷ Vofakilapo vinapangiwa na mkuwa. Vokobekapo na nkoli vinapangiwa na siliva, na vovininkila poika vinapangiwa na siliva. Vonse vochingilizila vinali vo vininkilika na siliva. ¹⁸ Nyula ya pongela muchochingilizila inali mikono twente kutalimpa. Nyula inali kuoneka yo buluwa, yofilila, na yofila, yotungiwa bwino, ndipo inali mikono twente kutalimpa. Inali mikono twente mukutalimpa na mikono faivi mukutalimpa kuyenda mumwamba, monga nyula za chochingilizila. ¹⁹ Inali na voikapo vili folo na vokobekako va siliva. Chovininkila pa mwamba pake na nkoli zake zinapangiwa na siliva. ²⁰ To kokomelelako hema ya chalichi na chochingilizilako tunapangiwa na mkuwa. ²¹ Ivi ndiye vintu vamene vinasebenza kupanga chalichi, chalichi ya chipangano cha malamulo, monga mwamene mose bana mu uza pachitenga. Inali nchito yaba levi mwamene anaba uzila itahama mwana mwamuna wa Aroni wa nsembe. ²² Bezele mwana mwamuna wa Uri mwana mwamuna wa Hur, waku mutundu wa yuda, anapanga vonse vamene mulungu ana uza mose. ²³ Oholiabi mwana mwamuna wa Ahisamaki, waku mutundu wa Dan, anasebenzela pamozi na Bezele mukupanga vobeza, monga woziba maningi, ndipo monga wotunga vo buluwa, vofilila, na vofila, na nyula zabwino. ²⁴ Yonse golide inasebenza kuchita nchito, mumalo yonse yogwilana na malo yoyela - golide kuchokela ku nsembe -inali twente naini na 730 tudunswa, to pimiwa mofunikila na malo yo yela. ²⁵ Siliva inpasiwa kuchoka ku bantu inali kulema handiledi imozi na 1,775 tudunswa, monga mu malo yoyela, ²⁶ olo meda imozi muntu aliyense, yojuba pakati, yopimiwa na kadunswa kamu malo yoyela. Iyi nambala inavomelezewa kulingana na bantu bonse bamene bana pendewa, banali na zaka twente -603,550 bamuna beka. ²⁷ Handiledi imozi yama siliva yana ikiwa pa malo yoyela na pansu pa mayula -Handiledi imozi, imozi pali ponse. ²⁸ Yamene yanasalako pa 1,775 tudunsawa twa siliva, Bezele anapangila tokobekelako, anavininkila pamwamba pa toikilapo, nakupangilako nkoli. ²⁹ Nsembe ya mkuwa yolema 2, 400 tudunswa. ³⁰ Anapanga pongenela mu hema yokumanilamo kusebenzesa ivi, guwa ya mkuwa, kabati ya mkuwa, vonse vosebenzesa vapa guwa, ³¹ munyansi mwa chochingilizilako, munyansi mwa pongenela mu chochingilizilako, tonse to popomelelako twa chalichi, na tonse to popomelelako twa hema twa chochingilizilako.

Chapter 39

¹ Naya blue, pepo, tonje ya reedi, bana panga nsalu zooneka bwino zo sebenzelako mumalo yo yela. Bana panga nsal ya Aroni yamu malo yoyela, monga Yehova analamulila Mose. ² Bazalo anapanga efodi ya goilde, ya b ulu, pepo, tonje ya redi, na nyula yo pepuka zibili-zibili. ³ Bana koma malata ya golide naku ya juba muma waya, kuya sebenze sa muli tonje ya bulu, pepo, na redi, namu manyula yo pepuka, chito ya ba kaswili. ⁴ Bana pangan vigawo vamumapewava efodi, vogwilana ku vili vamumakana yapa mwamba. ⁵ Chamumusana chopangiwa bwino chenzeli monga efodi; chenze chopangiwa na chigawo chiozi na efodi, yopangiwa na nyula zo pepuka zibili zibili yamene yenze golide, bulu, pepo, na redi, mongamwamne e Yehova analamulila Mose. ⁶ Bana konza myala za onyi, bana ika tofaka twa golide, yokonzewa na volemba kwati chozibililako nama zina yabana bamuna ba Isilayeli. ⁷ Bazalo anafaka magawo yama pewa ya efodi, kunkala myala yokumbukilapo kuli bana bamuna ba Isilayeli, Monga Yehova analamulila kuli Mose. ⁸ Anapanga gawo yapa chifuba, nchitoyaba kaswili vopanga monba efodi. Anavi panga na golide na bulu, na pepo, na tonje ya redi, na nyula yo pepuka. Inali yolingana konse konse. ⁹ Bana peteka nyula zapa chifuba pabili. 23 sentimita mu'utali na 23 sentimita mu'ufupi. ¹⁰ Bana ikamo mizela folo ya myala zamutengo. mizela yoyamba yenze na ya odemu, ya pitida, naya bareketi. ¹¹ Wachibili muzela wenze nayanfoki, ya safiro, na yahalomu. ¹² Wachitatu muzela wenze na lelmu na sibu, naya akalama. ¹³ Muzela wachifolo wenze na Tarsisi, ya sahamu ya yasefe. Vinaikiwa moikiwa golide. ¹⁴ Kunali myala zili twelovu, iliyonse nazina imozi yabana bamu a ba iliyonse yenze yodindiwa na zina yamutundu umozi mumitundu zili twelovu. ¹⁵ Pa nsalu yapachifuba bana panga munyolo monga ntambo, yomangiwa nagnide yabwino. ¹⁶ Bana panga ma kanzedwe yabili ya golide na mpete zibili, naku zigwilizana mpete zibili kuma kona ya nsalu zapachifuba. ¹⁷ Bana faka minyolo zomanga zibili za golide muma mpete yabili ku kona ya nsalu yapa chifuba. ¹⁸ Bana gwilanisana zinangu zibili kosilizila kwa vomabga va munyolo kuma konzedwe yabili. bana vigwilisana ku gawo yaku ma pewa ya efodi ngati pasogolo pake. ¹⁹ Bana panga mpete zibili za golide naku zifaka pali ma kona yabili yenamgu yansali zapa chifuba mu mbali mwamukati mwama lile. ²⁰ Bana panga futi mpete zibili za golide naku zigwilanisana kunyasi kwama gawo yabili yapama pewa yaku sogolo kwa efodi, pafupi na msoko pamwamba pa mumusana chopangiwa bwino a efodi. ²¹ Bana manga nsalu yapa chifuba na mpete zake kuma mpete ya efodi na ntambo ya bulu, kuti inkale yogwilana pa mwamba pa chamu musana chabwino cha efodi. Ivi venzeli chifukwa nyula yapa chifuba isa lekeko kuli efodi, ivi vinachitika monga Yehova analamulila Mose. ²² Bazalo anapanga mukanjo ya efodi nanyula ya bulu konse, nchito yabo tunga. ²³ Yenzeli na poseguka pongenesela muli pakati poseguka panali potungika mumbali mose kuto isangamwike. ²⁴ Pansi pamu soko, bana panga ma kanza ya bulu, pepo na redi na nsalu zo pepuka. ²⁵ Bana panga mabelo ya golide yoyela, naku faka ma belo pakati pama kanza kuzungulila kunyasi kwa mkano, pakati pamakanza. Belo namakanza- ²⁶ belo na makanza munyasi mwa mukanjo kuti Aroni atumikilemo. Ichi chinali monga Yehova analamulila Mose. ²⁷ Bana panga vovala pa mwamba nanyula yo pepuka va Aroni nava bana bake bamuna. ²⁸ Bana panga chisote chakumutu kusebenzesa nyula yo pepuka, vowamisa kumutu va nyula yo pepuka nsalu zovala mukati ya nyula yo pepuka, ²⁹ nachovala mumusana cha nsalu yo pepuka naya bulu, na pepo naya chingwe cha redi, nchito yabo tunga. ichi chinali monga Yehova analamulila Mose. ³⁰ Bana panga mbale yakolona yoyela nagolide yabwino, bana dindapo monga kulemba kwapa chidindo, "Oyela kuli Yehova." ³¹ Bana giwilanisana kulichovalakumutu na ntambo ya blue kumwamba kwa chovala kumutu. Ichi chenzeli monga Yehova analamulila Mose. ³² Manje nchito yamu kachisi, yamu hema yokumanila, insila. Bantu ba Isilayeli bana chita vonse. Bana konka malangizo yamene Yehova anapasa Mose. ³³ Banaleta kachisi kuli Mose-hema na vosebenzesa vonse mutanda, mafelemu, voimilila va kachisi na vapansi. Ku vininkila; ³⁴ kwavikumba vankosa vada ya redi, kuvininkila kwa kwachikumba cho pepuka, nama ketani kuti kubisike ³⁵ likasa ya umboni, nami tanda nachi valilo chachitetezo. ³⁶ Bana leta tebulo, viya vonse, namu mukate wo pezekapo; ³⁷ poimilila nyali ya golidde yoyela na nyali yake mumi zela, votandizila na mafuta yamu nyali; ³⁸ yachi golide guwa, mafuta yo zoela na vonunkilisa cholelemba chapa komo pongenela mukadisi. ³⁹ Guwa ya chisulo na bwalo ya chisulo natanda yake na viya na chidebe chitulu na chapansi chake. ⁴⁰ Bana leta cholelemba chapa bwalo nama pasita yake na vapansi, nama ketani yapakomo pongenela mukoti ntambo zake nama pegesi ya hema navonse vo sebenzesa pogwila nchito yamu kachisi, hema yokumanilamo. ⁴¹ Bana leta mukanjo wopangiwa bwino yosebenzelako mu malo yoyela mukanjo yoyela ya Aroni wa nsembe na bana bake bamuna kuti bagwile nchito ngati ya wansembe. ⁴² Pamene apo bantu bamu Isilayeli bana chita zonse nchiito monga Yehova analamulila Mose. ⁴³ Mose anafufuza nchito yonse, manje, onani, bana vichita. monga mwamene Yehova analamulila muli ichi bana chichita. Pamene apo Mose anaba dalisa

Chapter 40

¹ Pamene Yehova anakamba na Mose, kuti, ² "Pasiku yoyamba ya mwezi yoyamba chaka chanyowani ukakonzee kachisi, mu chihema chokumanilamo. ³ Ufunika kufakamo Likasayaumboni, ufunika kuchingiliza likasa na nsalu. ⁴ Ufunika kubwelesa tebulo na kuikapo vintu vonse vofunikila bwino vamene vipezekapo. Chokonkapo ufunika kubwelesa choikapo nyale naku yasha nyale. ⁵ Ufunika kuika guwa yansembe ya golide pa likasa ya umboni, anso ufunika kuikapo nsalu pa lobela mu kachisi. ⁶ Ufunika kuika guwa yansembe vo shoka ku sogolo ko ngenela kwa kachisi, chihema chokumanilamo. ⁷ Ufunika kuika chidishi chikulu pakati ka chihema yo sonkanilamo na guwa anso ufunika kuikapo manzi. ⁸ Ufunika kupanga mupanda bo yozungulila, anso ufunika ku pachikapo nsalu pa komo yamu panda. ⁹ Ufunika kutenga mafuta ozezela naku zoza kachisi na vonse vamene vipezeka mukati. Ufunika kuchipatula na vonse vipangizo kuli ine; pamene apo chizayela. ¹⁰ Ufunika kuzozoa guwa yansembe zopeleka na cipangizo vonse. Ufunika kupatula guwa kwa ine anso izankala yoyela kuli ine. ¹¹ Ufunika kuzuzya dishi ya bronzi na pansu na kuipatulila ine. ¹² Ufunika ku leta Aroni na bana bake bamuna kongenela ya chihema chokumanilamo anso ufunika ku basambika na manzi. ¹³ Ufunika kuvalika Aroni vovala vopatulika kuli ine, muzoze naku mupatula kuti atumikile monga wansembe wanga. ¹⁴ Mufunika kuleta bana bake bamuna na kubavaliika vovala. ¹⁵ Ufunika kubazoa mwamene wazozela ba tate bao kuti bani tumikile monga bansembe. kuzozewa kwao kuzabapangila ubusa wachikalile kufikila mibadwo ya bantu bonse." ¹⁶ Ndiye vamene Mose anachita; anakonkamvonse vamene Yehova anamu'uzua. anachita vintu vonse ivi. ¹⁷ Chakuti kachisi kana konzewa pasiku yoyamba yamwezi muchaka chibili. ¹⁸ Mose anapanga kachisi. anaika vonse malo mwake, nakazika makamwake, naimika mapulanga, namatanda, nausa mizati nz nsandamilaa zake. ¹⁹ Anayalika hema pamwa pa kachisi, naika chovininkila pamwamba pake, mwamene Yehova anamu'uzila. ²⁰ Anatenga vokambilila va chipangano naku ika mu Likasa. Anaika mitengo pa likasa na chotetezela pamwamba. ²¹ Anabwela likasa mu kachisi, anaikapo nsalu yo chingiliza likasa ya umboni, mwamene Yehova anamu'uzila. ²² Anaika tebulo muhema yokumanilamo, kumbali ya kumpoto kwa kachisi, panja pa nsalu. ²³ Anaika mukate pa tebulo pamenso ya Yehova, mwamdene Yehova anamulamulila. ²⁴ Anafika choikapo nyali mu hema yokumainilamo, pasogolo yatebulo, ku mwela ya kachisi. ²⁵ Anayasha malampu pamenso ya Yehova, mwamene mulungu enze anamulamulila. ²⁶ Anaika guwa ya nsembe yopyeiza ya golide muhrma yosankanilanamo kusogolo kwa nsalu. ²⁷ Anashokelapo nsembe zonunkila bwio, mwamene Mulungu analamulila. ²⁸ Anapachika nsalu pakomomya kachisi. ²⁹ Anaika guwa ya nsembe yo shoka pa komo ya kachisi, mu hema yokumanilanamo. Anaikapo nsembe yo shoka na nsembe yaunga, mwamene Mulungu anamu'uzila. ³⁰ Anafika dishi pakati ka hema yokumanilanamo na guwa, anaikapo manzi yosambila. ³¹ Mose, Aroni, na bana bake bamuna banasamba mumanja naku mendo yao muka dishi. ³² Ntawi iliyonse akayenda mu hema yokumanilanamo anso baka yenda ku guwa. Anali kuzisambika, mwamene Yehova anabauzila Mose. ³³ Mose anamanga mupanda ozunguluka kachisi an guwa. Anaika nsalu pakomo ya mupanda, munjila iyi, Mose anasiliza nchito. ³⁴ Pamene kumbi inavininkila chihema chokumanilanamo, anso ulemelelo wa Yehova unazaza kachisi. ³⁵ Mose sanakwanise kungena muchihema chokumanilanamo chifukwa kumbi ina unankalapo, na chifukwa ulemelelo wa Yehova unazula kachisi. ³⁶ Pamene paliponse kumbi ukachoka pa kachisi, bantu bamu Isilayeli banali kuyenda paulendo yao. ³⁷ Koma ngati kumbi siyi nachokepo pa kachisi, nishi bantu kunalibe kuyenda. Banali kunkala paka siku inaza nyamuliwa. ³⁸ Chifukwa kumbi ya Yehova inali pa kachisi ya muzuba, na mulilo wake unalipo usiku, pamenso ya bantu bonse bamu Isilayeli pa ulendo wabo onse.

Leviticus

Chapter 1

¹ Yehova anayitana Mose nakukamba na eve kuchokela ku hema yokumanilamo, kukamba kuti, " ² Kambani kuli bana ba Israeli nakubauza beve, ' Pamene muntu wina wa imwe abwela na chopeleka kuli Yehova, bwelesani monga nsembe yanu, ya n'gombe kapena gulu ya nyama zosunga. ³ ⁴ Ngati chopeleka ni chopeleka choshoka kuchokela kugulu ya n'gombe, afunika kupeleka imuna ilibe ulema. Afunika kupeleka pongenela ku hema yokumanilamo, kuti chinkhale chovomelesewa kuli Yehova. Afunika kufaka kwanja kwake pa mutu wa chopeleka choshoka, ndipo chizanhkala chovomelesewa kumbali yake kupanga chitentezo chake. ⁵ Pamene apo eve afunika kupaya n'gombe pa menso ya Yehova. Bana bamuna ba Aaron, a'nsembe, azalangiza gazi naku

mwaza paguwa yamene ili pongenela mu hema yokumanilamo. ⁶ Ndipo afunika kuchosa chikumba chazopeleka zochoka naku juba muvi gawo. ⁷ Ndipo bana bamuna ba Aaron wansembe baza ka mulilo pa guwa nakufaka bwino nkuni pa mulilo. ⁸ Ndipo bana bamuna ba Aaron, opeleka nsembe, bafunika kufaka vigawo, kufakilako mutu namafuta, pa nkuni zamene zili pa mulilo zamene zili pa guwa. ⁹ Koma vamumala na mendo afunika kusuka na manzi. Ansembe opeleka nsembe baza shoka vonse pa guwa yavopeleka voshoka. Izachosa fungo ya bwino kuli ine; chizanhkala chopeleka kupangila ine na mulilo. ¹⁰ Ngati chopeleka chapelekewa choshoka ku nyama zosunga, imozi pa mbelele kapena imozi pa mbuzi, afunika kupeleka imuna ilibe ulema. ¹¹ Afunika kuyipaya kumpoto kumbali ya guwa kuli Yehova. Bana bamuna ba Aaron, ba nsembe, baza mwaza magari yake kumbali yonse ya guwa. ¹² Eve ajube ichi muvigawo na mutu namafuta, ndipo wansembe afunika kufaka vigawo pa nkuni zili pa mulilo uli pa guwa, ¹³ koma vamumala na mendo vifunika kusuka na manzi. Ba nsembe bazapeleka vonse, nakushoka pa guwa. Nichopeleka choshoka, nakuchosa kafungo konunkila bwino kuli Yehovah; chizanhkala chopeleka kupangila Yehovah na mulilo. ¹⁴ Ngati chopeleka kuli Yehovah chinganhkale chopeleka choshoka cha tu nyoni, ndipo afunika kubwelesa chopeleka kapena olo nkunda ing'ono. ¹⁵ Ansembe afunika kuyi bwelesa pa guwa, nakuchosa mutu yake, nakushoka pa guwa. Na gazi yake ifunika kuchosewa kumbali ya guwa. ¹⁶ Eve afunika kuchosa voshangiwa na vamene vili nayo, nakuponya pabali pa guwa kumbali yaku mawa, mumalo ya milota. ¹⁷ Eve afunika kungamba mooneka ma papiko, koma asayigabanise pa bili. Ba nsembe bazashoka pa guwa, pa nkuni zili pa mulilo. Izanhkala nsembe yoshoka, nakuchosa kafungo konunkila bwino kuli Yehovah; chizanhkala chopeleka chopangiwa namulilo.

Chapter 2

¹ Ngati muntu aliyense aleta nsembe ya mbeu kuli Yehova, nsembe yake ifunika ku nkala flaulo yo salala, ndipo azatilako mafuta na kuika vo nunkila bwino. ² Afunika kupeleka nsembe kuli bana ba Aroni ba muna ba nsembe ndipo ba nsembe baza tengakapo ku zuzya kwanja flaulo yo salala ili na mafuta na vonunikila bwino, Ndipo wa nsembe baza shocka nsembe pa guwa monga bo imililako nsembe yo pasa kuli enve na mulilo. ³ Vili vonse viza salapo pa nsembe ya mbeu viza nkala va Aroni na bana bake bamuna. Nicho yela maningi kuli Yehova ku choka musembe kuli Yehova zo pangiwa namulilo ⁴ Ngati mwa peleka nsembe za mbeu zilibe vo fufumisa vamene va pikiwa mu uvuni, ifunika ku nkala mukate botoka ba flaulo ya salala yo sankaniza namafuta, olo mukate okosa ulibe vo fufumisa, omwazikana na mafuta. ⁵ Ngati nsembe zanu za mbeu za kazingiwa pa pani ya simbi, ifunika ku nkala ya flaulo yo salala ilibe vo fufumisa yo sankanizana namafuta. ⁶ Mugabanise mudunswa naku tililapo mafuta. Iyi ni nsembe ya mbeu. ⁷ Ngati nsembe yana ya mbeu ya ohikiliwa pa pani, ifunika ku pangiwa na flaulo yo salala na mafuta. ⁸ Mufunika kuleta nsembe za mbeu zo pangiwa kuli ivi vintu kuli Yehova, naku peleka kuli wansembe, wamene azaleta ku guwa. ⁹ Pamene apo wa nsembe azatengapo pa nsmeb ya mbeu moonga oyimililako wa nsembe, aku shoka pa guwa. Izankala nsembe yo pangiwa na mulilo ndipo iza chosa kafungo ka bwino kuli Yehova. ¹⁰ Vili vonse viza salapo pa nsembe ya mbeu vizankala va Aroni nabana bake bamuna. Nicho yela maninigi kuli Yehova ku choka munsembe kuli Yehova zo pangiwa na mulilo. ¹¹ Kulibe va nsembe va mbeu viza pasiwa Yehova viza pangiwe na vofufumisa, chifukwa musa shoke chotupisa kapena uchi, monga nsembe yo panga namulilo kuli Yehova. ¹² Muza vipasa kuli Yehova monga vopelelka vobadwa poyamba, koma sivilasebenzewa ku panga vo nunkila bwino pa guwa. ¹³ Mufunika ku ikako muchele ku chopeleka cha mbeu. musakaole muchele yachi pangano ya Mulungu wanu chosebeka mu vopeleka va mbeu. Na vopeleka vanu vonse mufunika ku pasa muchele. ¹⁴ Ngati muza pasa vopeleka va mbue vo badwa poyamba kuli Yehova, mupeleke mbue za fureshi vo shoka na mulilo naku pamunyilam mu vokudya. ¹⁵ Ndipo mufake mafuta na nsembe zo nunkila. Ichi nicho peleka cha mbeu. ¹⁶ Pamene apo wa nsembe aza shokapo chopeleka cha mbeu na mafuta na nsembe zo nunkila na chopeleka co imililka. Ichi ni chopeleka cho pangiwa kuli yehova.

Chapter 3

¹ Ngati winagu apeleka nsembe yamusonkano yamene iliyopeleka yanyama kuchokela mukola imuna kapena ikazi, afunika kupeleka nyama yamene ilibe choipa chilichonse pamenso ap Yehova. ² Azafaka manja yake pali mutu wachopeleka chake naku chipaya pa chiseko chahema yokumanilamo. Manje bana bamuna ba Aroni wa wansembe bazatilapo magazi yake mu mbali ya guwa. ³ Mwamuna azapeleka nsembe yamusonkano pa mulio kuli Yehova. mafuta yamene yavinikila olo kapena yogwilana muvigawa vamukati, ⁴ nama kidini yabili na mafuta yamene yalipo mumusana, mafuta ya liva, nama kidini-azachosa vonse ivi. ⁵ Bana bamuna ba Aroni baza vishoka ivo vamene ili pa nkuni zamene zili pamulilo. Ichi chiza chiosa mpepo yabwino ya Yehova; chizankala chopeleka chake chapa mulilo. ⁶ Ngati nsembe ya mwamuna yopeleka ya mumusonkano kuli Yehova niyo chokela munyama zusunga; imuna kapena ikazi, Afunika kupeleka chopeleka chili chonse. ⁷ Ngati apeleka nkosa kuti ndiye chopeleka chake, afunika ku ipeleka pamenso ya Yehova. ⁸ Azafaka manja yake pa mutu wachopeleka chake naku chipaya pasogolo ya hema yokumanilapo. Ndipo bana bamuna ba Aroni ba za tilapo magazi mu mbali ya guwa. ⁹ Mwamuna azapeleka nsembe yopeleka yamusonkano ngati chopeleka chopangiwa na mulilo kuli Yehova. Mafuta, mafuta yonse yakumudila kuyajubako pafupa yapakati pa musana, nama futa yamene yovinikila vigawo na yonse mafuta yamene yali pafupi navi gao vamukati, ¹⁰ nama kidini yabili na mafuta yamene yalinayo, yamene yalimu musana, napa mafuta ya liva, nama kidini azavichosa vonse ivi. ¹¹ Ndipo wansembe azavishoka vonse ngati nsembe yopyeleza kuli Yehova. ¹² Ngati chopeleka chamwamuna nimbuzi, ayi peleke pamensio pa Yehova. ¹³ Afunika kufaka maja yake pamutu wa mbuzi naku ipaya pasogolo ya hema yokumanilamo. Ndipo bana bamuna ba Aroni bazatila magazi mumbali ya guwa. ¹⁴ Mwamuna azapeleka nsembe yake yopangiwa mafuta yamene yavininkila magawo yamukati, namafuta yonse yalipafupi nama gawo yamukati. ¹⁵ Azachosa futi ma kidini yabili namafuta yamene yalinayo, yamene yali mumusana nama futa ya liva nama kidini. ¹⁶ Wansembe azashoka vonse pa guwa ngati nsembe yopyeleza ya chakudya kuchosa fungo yabwino. mafuta yonse niya Yehova. ¹⁷ Izankala lamulo yamuyaya pamibadwo yabantu bako bonse mumalo yali yonse yamene muzapanga nyumba kuti musadye mafuta kapena magazi."

Chapter 4

¹ Yehova anakamba kuli Mose kuti, ² "Bauze bantu baku Isilayeli, 'Ngati aliyense achimwa chosafuna kuchimwa, nakuchita vintu vamene Yehova analesa kuchita, ndipo ngati achita chintu chamene chilesdwa, ivi vamene vikonkapo vifuna kuchitiwa. ³ Ngati niwansembe wamene achimwa pakuti alengese bantu kupezeka wolakwa, ayenela kupeleka ng'ombe imuna yopempelelako chikululukilo ilibe kalema, kwa opeleka kwa Mulungu. ⁴ Ayenela kuleta ng'ombe imuna kutenti yamu sonkano pamaso pa Yehova, kusaufikapo manje pa mutu wake, ndi kupha ng'ombe pamaso pa Yehova. ⁵ Wansembe wozezewa azatengako ena mwa magari ya ng'ombe ndi kuyapeleka ku tenti yamu sonkano. ⁶ Wansembe azaika chikumo chake mumagazi ndi kumwaza gawo inangu kwelengela ka seveni pamenso pa Yehova, pafupi na nyula yamumalo yoyela maningi. ⁷ Wansembe azaika gawo inangu ya magari kunyanga za guwa ya nsembe kunyanga za guwa ya nsembe ya vofukiza vonunukila pamenos pa Yehova, yamene ipezeka mutenti yamu sonkano, ndipo azatila magari yonse yenangu yosalapo ya ng'ombe imuna pansi pamaziko ya guwa ya nsembe zowocha, yamene ipezeka polowela mu tenti yamusonkano. ⁸ Azachosako ma futa yonse ya nsembe yama chimo; mafuta yamene yama yaphima ziwalo zamukati, yonse mafuta yokangamila ku ziwalo, ⁹ Mphewo zonse na mafuta ya kangamilako. yamene yali mumusana na chima futa chaku chiwindi, na mpheo afunika kuchosako vonse ivi. ¹⁰ Azavijuwako vonse, monga mwamene amavijuwila kuchosa ku ng'ombe imuna ya chopeleka nsembe ya mutendele. ¹¹ Chikumba cha bg'ombe na nyama yosalako iliyonse, na mutu wake na mendo na vamukati vake vonse na matuvi yake. ¹² Viwalo vizasalako vinangu vonse va ng'ombe azanyamula vonse ivi viwalo kunja kwamunzi kupeleka kumalo kwamene auanyelesela ine, kwamene amatila maphulusa; azashokela ivo viwa pamene apo paukhuni. Afunika kushokela ivi viwalo pamene amatayila maphulusa. ¹³ Ngati wossankana wonse wa Isilayeli wachimwa chosafuna ku chimwa, ndi kuti osonkanawo saziwa kuti wachimwa na kuchita chintu pa vamene Yehova analamulila kuti visachitike na kupezeka na mulandu, ¹⁴ apo, pamene chimo yamene wanachita izaziwika, ndiye pamene osonkhanawo azapeleka ng'ombe ing'ono ya chopeleka cha chimo nakuileta pa tenti yamusonkano. ¹⁵ Asogoleli amusonkano azayika manja yawo pa ng'ombe pamenso pa Yehova, ndipo ng'ombe izapayiwa pamenso pa Yehova. ¹⁶ Wansembe wozozedwa azatenga mwa magari ya ng'ombe ku tenti yamusonkano, ¹⁷ ndipo wansembe azayika chikumo chake mu magari na kuyamwaza kali seveni pa pamenso Yehova kutilila kunyula yamutenti. ¹⁸ Azayikako magari yenangu ku nyanga za guwa yamene ili pamenso pa Yehova, mutenti yamusonkano, ndipo azatila magari yonse panyansi pa guwa yoshokelapo chopeleka, yamene ipezeka pongenela mutenti yamusonkano. ¹⁹ Azajuwako mafuta yonse nakuyashokan paguwa. ²⁰ Ivi ndiye vamene afunika kuchita na ng'ombe imuna. Monga mwamene anachitila na ng'ombe yachopeleka chachimo, ndiye mwamene azachitila na iyi ng'ombe futi, motelo wansembe azawaoangila chitelo wansembe azawapangila chitetezo wantu, ndipo azalandila chikhulukukilo. ²¹ Azaniyamula iyi ng'ombe kunja kwa munzi na kuyishoa monga ng'ombe yapoyamba ichi nichopele ka cha chimo cha wosonkhana. ²² Wolamulila akachimwa chosafuna kutiachimwe, nakuchitapo chimozi mwavintu vamene Yehova Mulungu analesa kuchita, ndipo apezeka wolakwa. ²³ pambuyo pake abwela aziwisiwa za chimo yamene anachita, afunika kupeleka mbuzi imuna ilibe kalema. ²⁴ Azayika manja pamutu pambuzi nakuyipayila mumalo mwamene amapayilamo nsembe yoshoka pamenso pa Yehova. ²⁵ Wansembe azatenga magari acha chopeleka chopepsela chimo na chikumo chake nakuyayika pa nyanga zaguwa yoshokela nsembe ndipo azatila magari yake yambili panyansi paguwa ya nsembe zoshoka. ²⁶ Azashoka mafuta yonse paguwa, monga chabe mwamene anashokela mafuta yachopeleka chamutendele. wansembe azapanga nsembe yachitetezo yochingiliza musogoleli mokuhuzana nachimo yake ndipo musogoleli azakhulukidwa. ²⁷ Ngati aliyense mwa bantu wamba achimwa chosafuna kuchimwa, achita chimozi mwa vintu vamene Yehova analesa kuchita, ndipo akaziwa kuti niwolakwa, ²⁸ manje ngati chimo yake yamene anachita yaziwika kuli mwine ndiye pamene azabwelesa mbuzi yopeleka nsembe yake yenve, mbuzi ikazi ilibe kalema, yopepsela chimo yamene anachita. ²⁹ Azayika kwanja kwake pamutu pa chopeleka chopepesela chimo nakupaya nsembe yopepesela chimo pamalo pamene amapelekela nsembe yoshouma. ³⁰ Wansembe azatengako magari yenangu nachikumo chake nakuya zoleka kunyanga za guwa ya nsembe zoshoka. Azatila magari yenangu yosalapo yonse munyansi mwa guwa yamene iti. ³¹ Azajuba naku chosako mafuta yonse, monga mwamene mafuta yama juwiwa naku chosewa ku chopeleka cha mutendele. wansembe izayishokela pa guwa kuti pachoke kafungo konunkila bwino kwa Yehova. Motero wansembe wapnga chotetezelako uja muntu, ndipo uyi muntu azakhulukidwa chimo yake. ³² Ngati muntu wabwelesa kamwana kambelele kuti kankale nsembe yopepeselako chimo yake, azabwelesa kakazi kamene kalibe kalema. ³³ Azayikapo kwanja kwake pamutu pa kankosa kopepesela chimo naku pepesela chimo mumalo mopyailamo nsembe yoshoka. ³⁴ Wansembe azatengako magari yenangu ya chopeleka chama chimo nachi kumo chake na kuyazoleka kunyanga zakuguwa yansembe yoshoka, ndipo azatila

magazi osala munyansi mwa guwa. ³⁵ Azachosako mafuta onse, monga mwamene anachosela mafuta, a kankhosa kuchokela ku chopeleka cha nsmebe yamutendele, ndipo wansembe azayashoka paguwa pamwamba pa zopeleka za Yehova zopangila ndi moto. Wansembe azamupangilako nsembe yomuombola kamba ka chimo yamene anachita, ndipo mwamunayo azakhululukiwa.

Chapter 5

¹ Ngati winangu wachimwa kamba kakusapeleka umboni pamene afunkila kutero, pa chintu chamene chenzo chitikiola mu menso mwake chamene afunikila kupeleka umboni, ² kapena anaonako kapena kumwelako chabe, azankala na mulandu. Kapena ngati winagu wagwira chili chonse chamene Mulungu amaciona chokowela, chingankale nthindi ya chinyama chokowela chamusanga mwina chokowela chamusanga mwina nthindi vokowela vamene uimayenda pansi, oko kuti sanaziwe vamene anachita, niwokokwela ndipo niwolakwa. ³ Kapena akagwila vadoti vawinangu, chokowela chilichonse, ndipo ngati saziwako kantu kai kpnse akabwela aziwa za ichi, apo ninshi azapezeka namulandu pantawi yamene aziwa vinachitika. ⁴ Kapena ngati winangu alapila mwilubilo na milomo yake kuti achite choyipa, kapena chabwino, chilichonse chamene muntu alapila mwa lubilo nanjazi, olo kuti sanaziwe za ichi, akabwela kuziwa za ichi, nishhi azapezeka namulandu, muli vamene ivi vamene tikambapo. ⁵ Pamene winangu apezeka niwolakwa muli ivi vintu, afunika kulapachimo iliyonse yamene anachita. ⁶ Chokonkapo afunika kuleta chopelaka chovomela mulandu kwa Mulungu choplapoila chimo yamene anachita, nyama ikazi yochokela paviweto, kankosa kapena mbuzi, yapepesela chimo, ndipo wansembe azamuchitla nsemne omuwombola kuchimo yamene anachita. ⁷ Ngati sangakwanise kugula kankosa, malo mwake anga bwelse monga ni chopeleka chovomelela mulandu tunkunda tuwili olo tuniwa tung'ono tuwili kwa Yehova, kozi ka chopeleka cha chimo ndipo kenangu ka chopelea choshoka pamulilo. ⁸ Afunika kuvileta kuli wansembe, wamene azapeleka kamozi kachimo poyamba -iye azakaponyongola mukozi pokachosa mutu kuthupi. ⁹ Chokonkapo azamwaza magari enangu ya chopeleka cha chimo kumbali kwa guwa. ndipo azafina magari osalomo munyansi mwaguwa ichi nichopeleka chopepesela chimo. ¹⁰ Apa manje afunika kupeleka ka nyoni kachiwili monga nsembe yoshoka, monga nsmebe yoshoka, monga mwamene chikambiwiwa mumalamulo, ndipo wansembe azapanga chipepeso chomuleselela ku chimo yamene anachita ndipo uyu mutnu azakhululukia machimo. ¹¹ Koma ngati sangakwanise kugula tunkhunda tuwili olo tuwana twa njiwa tuwili, ninshi afunia kubwelesa noimi wa fulawo yogaika bwinokupima ka teni ma efa yopangilako chopeleka cha chimo. Safunika kuyikako mafuta kapena zonunkiliza nsembe, pakati nichopeleka chopesela chimo ¹² Afunika kuileta kuli wansembe, na wansembe azatengapo mukwanja mwake muyeso wozula kwanja kuti inkale nemsbe yoyembekezelako ndipo azayishoka paguwa. pamwamba pavopeleka vopanga na mulilo kwa Yehova. Ichi nichopeleka chopepesela chimo. ¹³ Wansembe azapanga chotetezelako uja muntu pachimo iliyonse yamene anachita, ndipo uja mutnu azakhululukidwa. vosalako ku chopelekelako cha vamumunda. ¹⁴ Pamene apo Yehova anakamba na Mose, Kuti, ¹⁵ "Ngati muntu aliyense achimwa nakuchita mosakulupilila pa vintu va Mulungu, koma anachita iicho kosati mwadala, ndiye pamene afunika kuleta ch chopeleka chovomela mulandu kwa Yehova. Ichi chopeleka chifunika kunkala mbelele ilibe kalema yosankhulika ku chokela paviweto. mtengo wake muyenenla kupima siliva wapamwamba kupimmila pa sikelo yamutempile inkale nsembe yopepesa chimo. ¹⁶ Afunika kumukhutilisa Yehova pakapesedwe kukhuza vintu voyel, ndipo afunika kuyika mpimo wachi nambala faivi nakupasa wansembe. chokoukhapo wansembe azapeleka nsmebe yachitetzo kumupapatilako na mbelele yovomela chimo, ndipo uja mutnu azakhululukiwa. ¹⁷ Ngati aliyense wachita chimo naku chit chilichonse chamene Yehova analeza kuchita, olo kuti siyenze kuziwa ichi, niwolakwa kulakwa sochabe ndipo afunika kunyamula kulakwa kwake. ¹⁸ Afunika kuleta mbelele ilibe kalema kuchosa paviweto, kupima mutengo wambelele wamene uliko, manje, chinkale chopeleka chovomelelako mulandu kupeleka kuwansembe chokonkhapo wansembe azapeleka chpeleka chachipepeso kuchingilizako uja muntu ku chimo yamene anachita mosiziwa, ndipo azakhululukiwa. ¹⁹ Ichi nichopeleka chovomelako chimo, ndipo niwolakwa zo'ona pa menso pa Yehova."

Chapter 6

¹ Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, ² Munthu akachimwa, nachita mosakhulupirika kwa Yehova, mwa kupusitsa mnansi wake ndi kanthu kena kamsungidwe kake, kapena iye amene anasungidwa m'manja mwake, kapena za kanthu kena kalikonse kakuba, kapena ngati anazunza mnansi wake, ³ kapena iye wapeza chinthu chomwe mnzake wataya ndikunama, kapena ngati walumbirira zabodza, kapena pankhani ngati izi zomwe anthu amachimwa, ⁴ ndipo ngati wachimwa ndipo wapezeka kuti ndi wolakwa, ayenera kubweza chilichonse chomwe adamulanda mwa kuba kapena kuponderezana, kapena zomwe zidapatsidwa kwa iye, kapena zomwe zidatayika koma zomwe adazipeza. ⁵ Komanso, pa nkhanu iliyonse imene analumbirira monama, ayibwezere kotheratu ndipo aziwonjezera limodzi mwa magawo asanu a mtengo wake ndi kubweza zonse kwa mwiniwakeyo patsiku lomwe wapezeka wolakwa. ⁶ Kenako azibweretsa kwa Yehova nsembe yake ya kupalamula, nkhusa yamphongo yopanda chilema, yochokera pa ziweto zake, monga nsembe ya kupalamula kwa wansembe. ⁷ Wansembe aziphimba machimo ake pamaso pa Yehova, ndipo azikhululukidwa pa chilichonse chimene wachita. ⁸ Pamenepo Yehova ananena ndi Mose, nati, ⁹ Lamula Aroni ndi ana ake, kuti, Lamulo la nsembe yopsereza ndi ili: Nsembe yopsereza izikhala pa nkhanu za guwa la nsembe usiku wonse kufikira m'mawa, ndipo moto wa pa guwa la nsembeyo ukhale; kuyaka. ¹⁰ Wansembe azivala zovala zake, komanso atavala zovala zamkati. Iye azitola phulusa lotsala pambuyo pakuti moto wanyeketsa nsembe yopsereza paguwa lansembe, ndipo aziika phulusa pambali pa guwalo. ¹¹ Azivula zovala zake ndi kuvala zovala zina kuti anyamule phulusa kunja kwa msasa kumalo oyera. ¹² Moto pa guwa lansembe uzisungabe. Sayenera kutuluka, ndipo wansembe aziwotcha nkhanu m'mawa uliwonse. Aphimbe kaye nsembe yopsereza monga akufunira, ndipo adzafukiza mafuta a nsembe zoyamika. ¹³ Moto uziyakabe nthawi zonse paguwa lansembe. Sayenera kutuluka. ¹⁴ Ili ndilo lamulo la nsembe yambewu. Ana a Aroni azibweretsa izi pamaso pa Yehova patsogolo pa guwa lansembe. ¹⁵ Pamenepo wansembeyo atengeko ufa wokwanira wochuluka wa nsembe yambewu, mafuta, ndi lubani amene ali pa nsembe yambewu, ndipo aziwotcha paguwapo kuti zikhale fungo lokoma monga nsembe yoyimira. ¹⁶ Aroni ndi ana ake azidya zotsala za nsembeyo. Azidyera mopanda yisiti m'malo oyera. Azidyera pabwalo la chihema chokumanako. ¹⁷ Sayenera kuphikidwa ndi yisiti. Ndapereka choperekacho monga gawo lawo la nsembe zanga zotentha ndi moto. Ndiyo yopatulika koposa, monga nsembe yamachimo ndi nsembe yopalamula. ¹⁸ Amuna onse mwa ana a Aroni adyeko; Aliyense wokhudza zinthu zimenezi adzakhala woyera. ¹⁹ Pamenepo Yehova analankhulanso ndi Mose, nati, ²⁰ Iyi ndi nsembe ya Aroni, ndi ya ana ake aamuna, imene adzapereka kwa Yehova patsiku la kudzoza mwana wamwamuna; limodzi la magawo khumi la efa la ufa wosalala ukhale nsembe yaufa; , theka lake m'mawa ndi theka lake madzulo. ²¹ Awapanga ndi mafuta poto wophika. Mukamaviika, muziibweretsa. Muziipereka nsembe yambewu kuti ikhale fungo lokhazika mtima pansu kwa Yehova. ²² Mwana wa mkulu wa ansembe yemwe akukhala wansembe wamkulu watsopano pakati pa ana ake azipereka. Monga yauza kosatha, yonseyo izitenthedwere kwa Yehova. ²³ Nsembe yambewu iliyonse ya wansembe izitenthedwa ndi moto. Sayenera kudyedwa. ²⁴ Pamenepo Yehova analankhulanso ndi Mose, nati, ²⁵ Nena ndi Aroni ndi ana ake, ndi kuti, Ili ndi lamulo la nsembe yauchimo: nsembe yopepesera machimo iyenera kuphedwa pamalo pomwe nsembe yopsereza iphedwera pamaso pa Yehova. ²⁶ Wopereka nsembeyo chifukwa cha tchimo aziidya. + Azidyera m'malo oyera pabwalo la chihema chokumanako. ²⁷ Chilichonse chokhudza nyama yake chizikhala chopatulika, ndipo magazi ake ngati awazidwa pa chovala chilichonse, uwasuke, gawo lomwe anawaza pa ilo, m'malo opatulika. ²⁸ Koma mphika wadothi wophikiramo uyenera kuthyoledwa. Ngati yophika mumphika wamkuwa, iyenera kutsukidwa ndikutsukidwa m'madzi. ²⁹ Mwamuna aliyense pakati pa ansembe azidya ina chifukwa ndi yopatulika koposa. ³⁰ Koma nsembe yamachimo iliyonse, imene mwazi wake walowetsedwa m'chihema chokomanako kupepesera machimo m'malo opatulika, isadye; Chiyenera kuwotchedwa.

Chapter 7

¹ Iyi ndiye lamulo ya nsembe ya chopepesela mulandu. Niyoyela maningi. ² Bafunika kupaya nsembe yopepesela mulandu mumalo yake yopailamo, ndipo bafunika ku waza magazi yake kumbali yonse yozungila ya guwa. ³ Yonse mafuta yaa mukati yazapelekewa: mafuta, yakumuchila, ⁴ mafuta yali ku viwalo va mukati, Vibindi, namafyo-ivi vonse vifunika ku chosewa apa chibindi. ⁵ Wansembe afunika kushoka viwalo ivi pa guwa monga nsembe yoshoka kuli Yehova. Iyi ni nsembe yppesela mulandu. ⁶ Mwamuna aliyense pa bansenmbe anadyeko iyi nsembe. Ifunika kudyewa mu maka yoyela chifukwa niyoyela maningi. ⁷ Nsembe ya chimo ili monga nsembe yo pepesela mulandu imozi na imozi isebenza kuli vonse vibili. Nivawansembe wamene apanga vochingiliza navenve. ⁸ Wansembe wamene apeleka nsembe yo shoka ya muntu aliyense angatengeko va mumala vaija nsembe. ⁹ Nsembe iliyonse yambeu yamene yakazingiwa mu ovuni na nsembe iliyonse yopikiwa pa pani yokanzingila olo pani yopikilamo. Izankala ya wansembe oyipeleka. ¹⁰ Nsembe ya mbeu iliyonse inkale yoyuma olo yosankaniza na mafuta, nayenve izankala ya bpnse bobadwa kuli Aroni. ¹¹ Iyi ni lamulo yopeleka nsembe ya vamutendele yamene bantu bazapeleka kuli yehova. ¹² Ngati aliyonse aipeleka yoyamikila, pamene afunika kupeleka na nsmebe ya makeke yalibe chofufumisa, koma yosankaniza na mafuta, mukate yopangiwa mulibe vofufumisa, koma yotiliwa navmafuta na makeke yopangiwa nafulaulo yopepuka yosankanzia mafuta. ¹³ Anso palingo yopasa chiyamiko, afunika kupasa pamozi na nsembe yake yamutendele ya mukate ulina vofufumisa. ¹⁴ Afunika kupeleka imozi ya mutundu uyu pa vopeleka monga nsembe kuli Yehova. Izankala ya ba nsembe bamene ba waza magazi ya nsmeb yamutendele pa guwa. ¹⁵ Muntu yopeleka nsembe yamutendele chifukwa cha lingo yopeleka chiyamiko afunika nyama ya nsembe yake pa siku yopeleka nsembe. Safunikila ku siyapo kalikonse paka mailo. ¹⁶ Koma ngati chopeleka cha nsembe yake nichilango yolumbila, olo yalingo ya nsembe ya kuzisakila, nyama ifunika kudyewa pa siku yamene apeleka nsembe, koma vilivonse vizasalapo vinga dyewe ap siku yokonkapo. ¹⁷ Koma, nyama iliyonse ya nsembe yamene yasalapo pa siku ya chitatu izafunika ku shokewa. ¹⁸ Ngati, iliyonse nayama yopeleka ya mutnu yansembe ya mutendele yadyewa pa siku ya chitatu, siyiza landiliwa, kapena kubelengewa pa malo yawamene aipeleka. Izankala chintu chonyansa, na mutnu wamene azadya azatenga mulandu ya chimo yake. ¹⁹ Nyama iliyonse yogwila chintu cho sayela siyifunika kudyewa. Ifunika ku shokewa. Monga nyama nyama yonse, Aliyense oyela angadyeko. ²⁰ Mwaicho, muntu osayela wamene adyako nyama iliyonse yavopekana va nsembe ya mutendele ya Yehova-muntu uyu afunika ku jubiwa pa bantu bake. ²¹ Ngati aliyense agwila chintu chosa yela-ingankale ni muntu osayela olo nyama yosayela olo chili chonse shosayela ni chonyansa-ngati adyako kunya yopeleka ya nsembe ya mutendele ya Yehova, muntu uyu afunika ku jubiwa kuli bantu bake." ²² Pamene Yehova anakmaba kuli Mose, kuti, ²³ "Kamba ku bantu ba Isilayeli kuti, 'simufunika kudya mafuta ya ng'ombe, mbelele, olo mbuzi. ²⁴ Mafuta ya nyama yamene inafa siyinankale nsembe, olo mafuta ya nyama ya paiwa na vinyama va musanga, inasebenzesewa ku lingo inangu, koma simufunika kudya. ²⁵ Aliyense azadya mafuta ya nyama yamene bantu bapeleka monga nsembe kuli Yehova, uyo muntu afunika ku jubiwa ku bantu bake. ²⁶ Siufunika kudya magazi yaliyonse mu nyumba iliyonse yamu, ngankale niya nyoni ono nyama. ²⁷ Wamene azadya magazi yaliyonse, uyu muntu afunika ku chosewa pa bantu bake. ²⁸ Chakuti Yehova anakamba kuli Mose kuti, ²⁹ "Kamba ku bantu ba isilayeli na kunena kuti, "Wamene azapeleka chopeleka cha nsembe cha mutendele kuli Yehova afunika kupelekako chopeleka kuli Yehova. ³⁰ Nsembe ya Yehova yo shoka, manja yake ya zafunika ku ibwelesa. Afunika ku bwelesa mafuta na nganga, kuti ngamnga inga weyuliwe monga nsembe yoweyula pa menso pa Yehova. ³¹ Wansembe afunika ku shoka mafuta pa guwa, koma nganga izankala kuli Aroni na mubadwe wake. ³² Ufunika kupasa voyenelela kuli wansembe monga nsmebe yopeleka yo chokela musembe yake yamutendele. ³³ Wansembe, umozi wa mubadwo wa Aron, wamene apeleka magazi ya nsembe ya mutendele na mafuta-azankala na chintu choyenelela cha mbali yake ya nsembe. ³⁴ Chifukwa ninatenga kuchokela ku bantu ba Isilayeli, nganga ya nsembe yoweyula, na chibelo cha musonkano, ndipo va pasiwa kuli Aroni wa nsembe na bana bamuna monga mbali yawo ya ntawi zonse. ³⁵ Ichi nichogabiwa cha Aroni na mubadwe yake kuchokela ku nsembe ya Yehova yo shokewa, [a siku yamene Mose anabapeleka ku sebenzela Yehova mu nchito ya nsembe. ³⁶ Iyi ni guwa yamene yehova analamulila ku pasiwa ku chokela ku bantu ba Isilayeli, pa siku yamene anazoza ba nsembe. Iyi izankala guwa yabo nwati zonse mubadwo yonse. ³⁷ Iyi ndiye lamulo ya nsembe yoshoka, ya nsmebe yambeu ya chimo, nsembe yopepesela mulandu nsembe ya yoyelesela, na vopeleka va nsmebe yamutendele, ³⁸ Vamene Yaweh anapasa malamulo kuli Mose pa lupili ya Sinayi pa siku yamene analamulila bantu ba Isilayeli kupeleka vopeleka kuli Yehova muchipulu cha Sinyai."

Chapter 8

¹ yehova anakamba kuli Mose, kuti, ² "Tenga Aroni na bana bake ba muna, vovala namafuta yozozela, ng'ombe yachimuna yansembe yachimo, tubana twankosa tubili. basikiteti ya mukate ulibe vopakisa. ³ Bayike pamozi bonse bo sonkana pongrnela mutent yamisonkano." ⁴ Mose anachita vamene Yehova anamulamulila, ndipo bosonkana bana bwela pamozi pongenela mutenti yamisonkano. ⁵ Pamene apo Mose anakamba kuli bosonkana, "Ivi ndiye ve atilamulila Yehova kuit vichitike." ⁶ Mose analeta Aoni na bana bake bamu a noba sambika na manzi. ⁷ Anavalika Aroni mukanjo no mumanga ntanmbo mumusana, nakumu valika mukanji nomufaka chakumtu, nakumangilalila chakumutu na chopepuka chomanga mumusana nochimanga. ⁸ Anafaka chovala panganga, ndipo muchovala pachifubaq anafaka Urimu na Tumimu. ⁹ Anayika chisote pa mutu wake, napa chisote, nofaka mbale ya golide, na kolona yoyela, mwamene anamulamulila Yehova. ¹⁰ Mose anateng mafuta yoozezela, anazozeta malo yompempelelamo na vonse vinalimukati noz patulila Yehova. ¹¹ Anasnsa mafuta pa guwa kali seveni, anazozeka guwa na vonse vosebenzesa, chowashilamo nachapansi, kuzipatulila Yehova. ¹² Anatila mafuta yozozela pa mutu ya Aroni nomuzoza nakumupatulila Yehova. ¹³ Mose analeta bana bamua ba Aroni nakubavalika mikanjo. Anamanga ntambo mumusana yabo na nyula yotetela nakumupatulila Yehova. ¹⁴ Mose analeta ng'ombe imuna ya nsembe ya machimo, ndipo Aroni na bana bake bamuna bayika manja pa mutu ya n'omb e imuna yamene banaleta kusembe ya chimo. ¹⁵ Anaipaya motenga gazi noyifaka pasengo yapa guwa natukumo twake, kuyeleza guwa, anatila gazi pansa pa guwa, nokuyipatulila Yehova kuti ayiteteze. ¹⁶ Anatenga mafuta yonse yanali mukati, vovalila chiwindi, na mafyo yabili namafuta yabo, Mose anavishoka vonse paguwa. ¹⁷ Koma ng'ombe imuna, chikumba, nyama, na matuvi yang'ombe, anavishoka panja pa musonkano, mwamene anamulamulila Yehova. ¹⁸ Mose anapeleka kamwana kankosa pa nsembe yoshokelaa, Aroni na bana bake bamuna banaika manja yabo pa mutu pakamwana ka nkosa. ¹⁹ Anakapaya naku sansa magari kumbali konse kwa guwa. ²⁰ Anajuba kamwana ka nkosa muviduswa duswa naku shoka mutu navidunswa nama futa. ²¹ Anasuka vamukati na mendo kusebenzesa manzi, ndipo anashoka kamwana ka nkosa konse pa guwa, Inali nsembe yoshika ndipo inachosa kafungo kabwino, nsembe yopangiwa na mulilo kuli Yehova mwamene Yehova analamulila Mose. ²² Mose anapeleka kamwana ka nkosaa kenangu, ko konzela, ndipo Aroni nabana bake banayika manja yabo pamutu yaka mwana ka nkosa. ²³ Aroni anakapaya, Mose anatenga magari noyika kumbali kwa guwa kwa kwatu ya Aroni yaku zanja lamanja, pachikumo chaku zanja lamanja. ²⁴ Analeta bana ba Aroni bamuna, nakufaka magari pa kwatu zanja lamanja, pachikumo chakuzanja lamanja, na pachikumo chikulu chaku kwendo kwaku zanja lamanja. Ndipo Mose anasansa kumbali konse kwa guwa. ²⁵ Anatenga mafuta, mafuta yakumuchila namafuta yonse yanali yamukati, vovala chiwindi, mafyo yabili namafuta yabo, kwendo kwaku zanja lamanja. ²⁶ Kuchokela mu basiketi yamukate ulibe vofufumisa inali pamenso ya Yehova, anatenga mukate umozi ulibe vofufumisa, na mukate unali nama futa umozi, namukate yopepuka, nozifaka pa mafuta napa kwendo kwaku zanja lamanja. ²⁷ Anavifaka vonse mukwanja kwa Aroni namumanja ya bana bamuna ba Aroni nakuviweyula pamenso ya Yehova kukala nsembe yoweyula. ²⁸ Pamene apo Mose anavichosa mumanja mwao nakuzi shoka pa guwa ya nsembe yoshoka. Inali nsembe yonkozekele inachosa naka fungo ka bwino. Inali nsembe yopangilana mulilo kuli Yehova. ²⁹ Mose anatenga nganga naku iweyula kunkala nsembe yoweyula pamene ya Yehova. Nkosa inalimbali ya Mose pa kunkazikisa, mwamene analamulila Yehova. ³⁰ Mose anatenga mafuta yozozela na magari yanali pa guwa; anavisansa pali Aroni, pavoala vake, pa bana bake, pavoala vabana bake. Munjila iyi anapatula Aroni na vovala vake, na bana bake na vovala vabo kuli Yehova. ³¹ Mose anakamba kuli Aroni na bana bake, "Pikani nyama pongena mu tenti ya musonkano, nokudya pamene paja namukate uli basiketi yokozela, mwamene analamulila kuti Aroni na bana bake bazakadya. ³² Vamene vikasalako kunyama na mukate muzafunika kushoka. ³³ Simufunika kuchoka pongenela mu tenti yamisonkano kwama siku yali seveni, kufikila masiku ya kuzoza yaka kwanile. Yehova aza mikonza mokwanila masiku yali seveni. ³⁴ Vamene vachitika lelo-Yehova alamulila kuti vichitike kuteteza kuli imwe. ³⁵ Muzankala muzuba na usiku kwa siku yali seveni pongenela mu tenti yamisonkano, nakusunga ma lamulo ya Yehova, chakuti musafe, chifukwa ivi ndiye vamene nina lamulila." ³⁶ Chakuti Aroni na bana bake bamuna banachita vamene anaba lamulila Yehova kupitila muli Mose.

Chapter 9

¹ Siku ya nambala eiyyiti Mose anaitana Aroni na bana bake bamuna na bakulu bamu Isireli. ² Anakamba kuli Aroni, "Tenga ka ng'ombe ka ng'ono pa gulu ya ng'ombe ka nkale ka nsembe ka chimo, naka mwana ka nkhusa kalibe chilema ka nkale ka nsembe koshoka, muzibwelese pamaso ya Yehova. ³ Ukambe na bantu baku Isireli naku kamba kuti, Tengani mbuzi imuna inkale nsembe ya chimo naka mwana ka ng'ombe na mbelele, zonse na zaka imozi ndipo ilibe chilema, inkale nsembe yo ocha; ⁴ anso mutenge ng'ombe na nkhusa kuti inkale chopeleka cha mutendere pamaso ya Yehova, na mbeu yosanganiza mafuta, chifukwa lelo Yehova azaonekela kuli imwe". ⁵ Pamene apo bana leta vamene anaba lamulila Mose ku chihema chokumanilapo, namusonkano wonse wa Isireli unavendela pafupi naku imilila pamaso ya Yehova. ⁶ Mose anakamba kuti, " Ivi ndiye vamene analamulila Yehova kuli imwe kuti muchite, kuti ulemelelo wake uonekela kuli imwe." ⁷ Mose anauza Aroni, " Bwela pafupi na guwa kuti upeleke cha chimo yako na choshoka chopeleka, naku zipangila chitetezo chako, na bantu, naku peleka nsembe ya bantu kuti ubapangile chitetezo chabo, monga mwamene Yehova analamulila." ⁸ Pamene apo Aroni anayenda pafupi na guwa naku paya ka mwana ka ng'ombe huti ka nkale kopeleka ka chimo, yamene inali yake. ⁹ Bana bamuna ba Aroni banazi onesela magari kuli yenve, anadinizamo ka kumo kake, nakufaka ku nsengo yaku chi guwa; naku tila magari pansi pa guwa. ¹⁰ Koma, anashika mafuta, mpafu, navo vininkilako liver pa guwa yopelekelako pelekelo ya chimo, monga mwanene analamulila Yehova kuli Mose. ¹¹ Nyama na chikumba anashokela panja pa munzi. ¹² Aroni anapaya yoshoka pelekelo, anso bana bake bamuna banamupasa magari, yamene anamwaza kumbali kwa guwa. ¹³ ndipo bana mupasa vopeleka voshoka, vojuba juba, pamozi na mutu wake, naku vishoka pa guwa. ¹⁴ Anasuka vamu kati na mendo naku shokela pamwamba pa vopeleka vo shoka pa chi guwa. ¹⁵ Aroni anaionesa nsembe ya bantu -mbuzi, naku ipeleka nsembe yama chimo yabo naku ipaya; anaipoleka ya chimo, monga mwamene anachitila na mbuzi yoyamba. ¹⁶ Anaionesa pelekelo yoshoka naku ipeleka monga mwamene Yehova analamulila. ¹⁷ Anapeleka mbeu yopeleka; anazulisa kwanja yake naku shoka pa guwa pamozi nayo peleka yoshoka ya kuseni. ¹⁸ Anapaya ng'ombe na nkhusa, nsembe yopeleka ya mutendele, yenzeli ya bantu. Bana ba Aroni bamuna bana mupasa magari, yamene anawaza pa guwa. ¹⁹ Mwaicho, anachosanmafuta mu ng'ombe imuna na nkhusa, muchila vamukati, mphafu, na yovinikila liver. ²⁰ Anatenga vamene banajuba naku vifaka pachifuba, naku shoka mafuta pa guwa. ²¹ Aroni anaweyula ngangazo na kwendo kuti inkhale ngangazo yopeleka pamaso ya Yehova, Monga mwamene analamulila Mose ²² Aroni ananyamula manja yake kuli bantu; pamene apo anabwela pansi kuchoka ku peleka pelekelo ya mutendele. ²³ Mose na Aroni bana yenda mu chihema chokumanilamo, banachoka futi naku ba dalisa bantu, na ulemelelo wa Yehova unaoneka kuli bantu bones. ²⁴ Mulilo unachoka pamaso ya Yehova nakudya vokudya voshoka vopeleka na mafuta pa guwa. pamene bantu pamene bantu banaona ivi, bana punda naku gona nfeshi ilangana pansi.

Chapter 10

¹ Nadabi Na Abihu, bana bamuna ba Aroni, aliyense anatenga lubani, nakuikamo mulilo, na vonunkila bwino vopeleka nsembe. Manje banapeleka mulilo osavomekezewa kuli Yehova, wamene sana lamulile kuti bapeleke. ² Chakuti mulilo unachoka kuli Yehova na kubaononga benve, nakufa pamenso pa Yehova. ³ Pamene apo anakamba kuli Aroni, "Ivi ndiye vamene Yehova analikukambapo pamene anakamba kuti, 'Niza onesa pafupi naine. Niza pasiwa ulemelelo pamenso pa bantu bonse.'" Aroni sanakambe vintu vili vonse. ⁴ Mose anaitana Mishael na Elzafan, bana bamuna Uzziel malume wa Aroni, ndipo anakamba kuli benve kuti, "bwelani kuno ndipo mutenge balongo banu kuba chosa monumanila popemphelela." ⁵ Chakuti banabwela pafupi naku batenga, banali bakali bovala va nsembe, kuchoka mofumanila, monga mwamene Mose anabauzila. ⁶ Pamene apo Mose anakamba kuli Aroni na Eleazar na Ithamar, bana bamuna bake, "Musaleke sisi mumitu zanu kunkala zosa sakula, ndipo osang'amba zobvala zanu, futi musafe, na kuti Yehova asakalipile gulu yonse. Koma osalola ba banja banu, nyumba yonse ya Isilayeli, kulila bonse bamene mulilo wa Yehova washoka. ⁷ Musayende pochokela mokumanilana, kapena muzafa, chifukwa mafuta yozozela ya Yehova yali pali imwe." Ndipo anachita kulingana na chilangizo cha Mose. ⁸ Yehova anakamba kuli Aroni, Kuti, ⁹ "Osamwe vinyu kapena moba ukali, iwe, kapena bana bamuna nako bamene basala naiwe, pakuyenda mokumanilana, futi usafe. Ichi chizankala chilamulo chamuyaya mu milondo zabantu bako, ¹⁰ kusiyanisa pakati pa oyela na bantu chabe, na pali osayela na oyela, ¹¹ chakuti unga punzise bantu bonse banu Isilayeli chilamulo chamene Yehova alamulila kupitila muli Mose." ¹² Mose anakamba Aroni ana Eleazar na Ithama, bana bake bamuna banasalapo, Tengani nsembe yachakudya yamene yasalapo ku nsembe ya Yehova yamulilo, ndipo mudye kulibe chopasikila mumbali mwa guwa, chifukwa ndimwe oyela kwambili. ¹³ Ufunika kudyela mumalo moyela kwabil, chifukwa ni chigawa chako na chabana bako bamuna ya nsembe ya mulilo ya Yehova, Pakuti ivi ndiye vamene nalamulila kuti nimu'uzeni. ¹⁴ nganga yoweyula na kwendo yopeleka kuli Yehova, ufunika kudya pamalo yovomekezewa kuli Mulungu. Iwe na bana bako bamuna na bana bakazi naiwe mudye muzingao, pakuti vipasiwa kuli iwe mogabiwa bana bamuna bako bamogabila chopeleka nsmebe mukukumana kwabantu baku Isilayeli. ¹⁵ Kwendo yopeleka na nganga yoweyula, yafunika kubwelesa nsembe zamafuta zopangiwa namulilo, kuweynula kuli Yehova. vinkale vako na bana bamuna bako muzagabana mwamuyayaya. ¹⁶ Pamene apo Mose anafunsa pali mbuzi ya nsembe yama chimo, ndipo anapeza kuti yoshokewa ndipo ana kalipa Eleazar na Ithamar, bana bamuna ba Aroni; Anakamba kuti, ¹⁷ "Nichani simunadye nsembe ya chimko mumala opephelela, pakuti ndiye malo oyela, na pakuti Yehova akupasani ichi kuti uchimo pamalo okumanilapo uchosewe, kunkala chitetezo pamaso pake? ¹⁸ Onani, magari siyana bwelesewe mumalo opephelelamo, ndipo imwe mucho'onadi simunade mumalo opephelelamo, monga ine ninalamulila." ¹⁹ Pamene Aroni anayanka Mose kuti, "Ona, lelo bapanga nsembe yama chimo yabo na nsembe yoshoka pamenso ya Yehova, ndipo ichitnu chachitika lelo kuli ine. Ngati ninali nadya nsembe yama chimo lelo, nga chinalai chokondwelesa mumenso ya Yehova?" ²⁰ Pamene Mose ananvela ivi, anali akutula.

Chapter 11

¹ Yehova anakambisana na Mose na Aroni, kuti, ² "Kamba kubantu ba Isilayelu, kuti, ivi ndiye vintu vamoyo vamene mufunika kuya pa vinyama vonse vamene vili paziko. ³ Mungadye nyama iliyonsr yamene ilina chodyakila chopatulikana ndipo yamene imgaya nakudya vamumala. ⁴ Koma, olo nitelo vinyama vinangu vimadya vamumal vikagaya kapena vili na chodyakila chogawanika, ndipo simufunika kuvidya, vinyama vogeya koma ilibe chibodo chogawikana, motelo kamelo niyodyesedwa kwa imwe. ⁵ Ndiponso chinyama chamumyala, chifukwa chimasheta vogaya koma chilibe chodyakila chogawikana, nichokowela nachenve kwa imwe. ⁶ kakalulu, chifukwa kakudya vogaya, koma kalibe chibodo chogawikana, nikadothi kwa imwe. ⁷ Nkumba olo ili na chibodi chogawikan koma siyimdy vogeya, niyo kowela kwa imwe. ⁸ Osadya nyama yawo iliyonse, kapena kukumyako nthindi zawo. nivokowela kwa imwe. ⁹ Vinyama vonkala mumnazi vamene mufunika kudya nivija vamene vili na chipyemohye chonyayilako namamba, munynaja yayikulu kapena mumusinje. ¹⁰ Koma vinyama vamoyo vamene vilibe tonyayilako namamba mu nyanja yayikulu kapena mumana, kuyikako vonse vamene viyenda memanzi kuyikako vamoyo vonse vamene vinkala mumanzi muzinyansidwa navo imwe. ¹¹ Pakuti mufunika kuvizondaa, osadya nyama yabo; futi, nthindizawo muzonde. ¹² Chilichonse chsmene chinkala mumanzi koma chilibe chipyempyme na mamba nichonyansa kuli imwe. ¹³ Ivi ndiye vmene mufunika kunyansiwa navo- ndipo simufunika kuvidya chifukwa nivonyansa; nkazi makubi, ndi makubi ya bulaki, ¹⁴ kayite, mutundu ulionse vinyoni vokudya vinzanke, ¹⁵ Mtundu uliwonse wa makwangwala, ¹⁶ kazizi wa nyanga ndi kazizi wamaloza, bakha mwamumazni, namutundu ulionse wavinyo i vokudya vinzake. ¹⁷ Mufunika kunyansiwa nakazizi wamung'ono ndi kazizi wamukulu ndi makonongo, ¹⁸ Kazizi woyela, ndi kazizi wakunkhokwe, nkawzi yakumanzi, ¹⁹ nyoni zakudya mapil, mdundu ulionse wa nkawzi zaku maiko akutali. nyoni zobo, ola mutengo, ndi nyankhupiti. ²⁰ Nthete zonse zamapiko zamene zi mayenda pa mendo folo ndizo nyana kwa iwe. ²¹ Koma mungadye nthete zowuluka zilizonse zamene ziyeda pamendo folo ngati vili namendo yolundikana pofuna kundalala. ²² Ufunika kudya mutndu ulionse wazombe, chigulugufe, nthete yojumpha, apena chidiza. ²³ Koma vidoyo vombuluka vonse vamendi folo ufunika kunyansidwa navo iwe. ²⁴ ²⁵ Uzankala wokowela mpaka ku mazulo na ivi vamoyo ngati ugwiila nthindi zawo, moziwawo. Aliyense wamene azadoba mathupi ya ivi vamoyo afunika kuwasha zovala zake ndipo ankhala okowela mpaka mazulo. ²⁶ Nyama iliyonse yamene ili na chibodo chogwaikana koma sichogewikilatu olo yamene siyimadya vogeya ili yokowela kwa iwe. Aleyense wamene azavigwila azankala wokowela. ²⁷ Chilichonse chamene chima yendela pa tukuma pavinyama vonse vamene viyenda namendo folo, nivodesedwa kwa imwe. ²⁸ Aliyense wamene azagwila nthindi yamutndu wanyama izi azakowela mpaka mumazulo. Aliyense wamene azanyamula thupi ya mtundu uyu wavinyama afunika kuwasha zovala zake ndipo azankala wokowela mpaka mumazulo. Ivi vinnyama vizankala vodesedwa kwa imwe. ²⁹ Pavinyama vamene vikalawa pasni, ivini nyama vamene vizankala vokowela kwa imwe, kaudende, koswe, ³⁰ na mutundu ulionse wa malinso wakulu, sosomezo, mbululu, gumu gumu, buluzi wamamba, ndi lumvwi. ³¹ Pavinyama vonse vamene vinkala, ivi nivinyama vamene vizankala vokowela kwa imwe. Aliyense wamene azagwila vinyama ivi pamene vili vakufa, azakowela mpaka mumazulo. ³² Ngati imozi mwavinyama ivi yafa naku gwela pa chintu chili chonse icho chintu chizakowela, olo nichinpanga na maplanga, chovala, chikumba, kapena chovala chamasaka oko nichabwanji loko kuti wama chisewenzesa munjila bwanji, chifunika kuyikiwa mumanzi, chizankala chokowela mpaka mumazulo. Ndiyr pamene chizankala choyela. ³³ Pakuti mpoto yowemba iliyonse yamene pazagwela, mukati olo kunja, chinyama chokowela, chilichonse chamene chili mu poto chizauduka chokowela, ndipo muyenela ku upwanya ija mpoto. ³⁴ Chakudya chilichonse chamene chinga dyewe koma chili namanzi yowazikilako kuchokela mu mpoto yamusango uyu, ninshi chakowela. ³⁵ Chilichonse chamene nyama yawo izagwelapo chisauduka chokowela ngati ni oveni kapena kasitovu kang'ono, chiyenela kupwaniwa mutudunswa. Nivokowela ndipo vifunka kunkala vokowela kwa iwe. ³⁶ Nyeuja kapena mugodi wotopapo manzi imankhalila yoyela koma aliyense wamene azagwila nthindi zace aliwodesedwa. ³⁷ Ngati gawo iliyonse yanyama izi yagwela pa mbweu yoshanga, izi mbeu zikali zoyela. ³⁸ Koma ngati manzi yazaikiwa pa mbeu, ndipo gawo iliyonse ya izinyama yagwelapo, ndiye kuti izi mbeu zizankhala zokowela kwa iwe. ³⁹ Ngati nyamaniliyonse yamene imwe mumadya yafa, ndiye kuti aliyense wamene akumyako mathupi ya nyama izi azankala wodesedwa mpaka mumazulo. Aliyense wamene azadya ija nyama afunika kuwasha vovala vake na knkala oowela mpaka mumazulo. ⁴⁰ Aliyense wamene anyamula nthindi yamutundu uyu azawasha zovala zake nakunkala wokowela mpaka mumazulo aliyense wamene azanyamula nyama yamutundu uyu azawasha zovala zake ndu kunkala wokowela mpaka mumazulo. ⁴¹ Nyama iliyonse yamene ikawala pasni niyonyansa osadya. ⁴² Chilichonse chamene chikalaba pamala pake, ndipo chilichonse chamene chiyendela pa mendo yake yali folo yonse, olo chilichonse chamene chilinamendo yambili vonse vinyama vamene vikalawa pasni ivi osadya, pakuti

nivonyansa. ⁴³ Osazikowesha mweka na chinyama chamoyo chilichonse chamene chiyenda pansi chokalawawa; osazikowesha nayenve pakuti viku pangenj osalungama. ⁴⁴ Pakuti ine ndine Yehova Mulungu wanu, Muyenela kuzisunga mweka oyela, Motelo, nakunkala oyela, chifukwa ine ndine woyela Osazikowesha mweka na mtundu ulionse wa nyama chamene ziyenda yenda pansi. ⁴⁵ Pakuti ndine Yehova, wamene anaku chosani kunja kwa ziko ya Iguputo, kuti ninkale Mulungu wanu. Nichifukwa chake muyenela kunkala oyela, pakuti ndine oyela. ⁴⁶ Iyi ndiye lamulo lonela zavinyama, vinyoni, ndi chamoyo chilichonse chamene chiyenda mumanzi, na cholengewa chamoyo chilichonse chamene chiyenda pa ziko, ⁴⁷ pakuti pafunika kuikapo kusiyanisa pakati pa vokowela navosakowela, na pakati pa vintu vamoyo vamene sivingadyewe."

Chapter 12

¹ Yehova anakamba kuli Mose, ² 'Kamba na bantu baku Isireli, ngati mukazi afika pakati naku bala mwana mwamuna, azankala wadothi masiku yali seveni, monga masiku yamene aliku mwezi. ³ Siku ya namba eyiti badule nkanda yaku sogolo kwa umuna. ⁴ na kuyeresa kwa magari yaba mai luza pitiliza masiku yali theti thri. asa gwile chili chonse chopatulika olo kubwela mu malo ya chihema paka masiku ya kuyeresa. ⁵ Koma akabala mwana mukazi, azankala na doti masiku fotini kulingana na masiku yake yaku mwezi. Kuyera kwa mai kuza pitiliza masiku yali sikiste sikisi. ⁶ Pamanene masiku yake yoyeresa yasila, kapena mwana mwamuna olo mukazi, azafunika kuleta ka mbelele kazaka imozi kuti ka nkale kopeleka ko shoka, naka nkund ka mwana kuti ka nkale ko peleka ka chimo, pongenela mmu hema yokumanilamo, kuli abusa. ⁷ kuchoka apo azapeleka kuli Yehova naku panga chitetezo=ero yayenve, naku muklina kuli magari yakugwa kuli enve. ndiye lamulo yo yakuli mukazi abal mwana mwamuna olo mukazi. ⁸ Ngati sakwanisa mbelele, ninshi apeleke nkunda zibili. imozi pelekelo yoshokewa inangu yachimo., kuchokapo abusa azamuoangila chitetezo; kuchoka apo azankala oyera.

Chapter 13

¹ Yehova anakamba kuli Mose na Aroni, kuti, ² "Ngati aliyense pa nkanda ya patupi yabo alina chovimba olo chituzo olo kapena chibamba, ndipo chankala na matenda yakuate pa nkanda ya tupi yake, chifukwa chake afunika kuletewa kuli Aroni mukulu wansembe, olo kuli mwana wake umozi wansembe. ³ Pamene wansembe azaona matenda pa nkanda ya patupi. Ngati sis p malo pali matenda ya sanduka yoyela, ngati matenda yaboneka yopitila pa nkanda, ndipo iyo ni matenda ya kate. wansembe akamuona, afunika kuitawa odesedwa. ⁴ Ngati chibamba chotuba pa nanda yake cho yela, ndipo kaonekedw sikapilila mkanda, ngati sisi malo ya matenda sina sanduke yoyela, Ndipo wansembe afunika kuchosapo uja ali namtenda masiki seveni. ⁵ Pasiku ya seveni, wansembe afunika kuona ngati mukuona kwake matenda siyana pitilile, ngati siyana pitilile mu nkanda. Ndipo wansembe afunika kumupatul masiku seveni pamwamba pake. ⁶ Wansembe aza muonanso pasiku ya seveni kuona ngati matenda yali bwino ndipo siyana pitilile mu nkanda. Ngati siyana pitilile, ndipo wansembe azamuitana kuti ndi oyela, ni vimpele. Afunika kuwasha vake, ndipo ni oyela. ⁷ Koma ngati vimpele vapitiliza mu nkanda pambuyo pozionesa kuli wansembe pa kuyela kwake, iye afunika kuzi onseanso kuli wansembe futi. ⁸ Wansembe azamuona kuona ngati vimpele vapitilila mu nkanda. Ngati vapitilila, ndipo wansembe afunika ku muitana kuti odesedwa. Ndimatenda yo yambukila. ⁹ Ngati matenda yo yambulila munkanda muli wina, afunika kuletewa kuli wansembe. ¹⁰ Wansembe azamuona kuona ngati pali chovimba choyela pa nkanda, ngati sisi yasanduka yoyela olo ngati pachovimba pal munyofu. ¹¹ Ngati ilipo, ayo nimatenda yakele yapa nkanda, wansembe afunika ku muitana kuti odesedwa saza mu chosapo, chifukwa ni odesedwa kale. ¹² Ngati ntenda iyi yayambukila mu tupi na kuphimba nkanda yonse ya muntu ali matenda kuyambila kumutu naku mapzi, monga mwane aonela wansembe, ¹³ Ndipo wansembe afunika ku muona ngati matenda ya phimba tupi yonse. Ngati ya phimba, ndipo wanse, be afunika kuitana uja muntu ali namatenda kuti oyela. Ngati yonse yasanduka yoyela, iye ndi oyela. ¹⁴ Koma ngati munyofu wofila waonekela pali enve, azankala odesedwa. ¹⁵ Wansembe afunika kuona pali munyofu wofila ndi kuitana kuti odesedwa chifukwa munyofu wofila ni odesedwa. Ndiye matenda yoyambukila. ¹⁶ Koma ngati munyofu wofila wankalnsa wouela, uyo muntu afunikila kuyenda kuli wansembe. ¹⁷ Wansembe azamuona kuona ngati nkanda ya sanuka yoyela, Ngati sanduka yoyela wansembe azaitana muntu uja kuti ni oyela. ¹⁸ Ngati muntu ali nahilonda pa nkanda yake ndipo chapola, ¹⁹ ndipo mumalo yachilonda pa nkanda yake ndipo chibamba chotuba, chotuluka, chifunika ku onesewa kuli wansembe. ²⁰ Wansembe azachiona kuona ngati chioneka chopitilila pansi pankanda, ngati sisi yasanduka yoyela, ngati zili motelo, wansembe azaitana uja muntu kutio wodesedwa. Ndi ntenda yoyambukila, ngati ya yamba pa malo penze chipumba. ²¹ Koma wansmbe akachiona na kuuona kuti mulibe sisi yoyela muli enve, ndi kuti sichili pansi pa nkanda koma chsilila, ndipo wansembe afunika ku muchosapo iye masiku seveni. ²² Ngati chayambukila maningi, pa nkanda, ndipo wansembe afunika kumuitana kuti wodesedwa ni matenda yo yambukila. ²³ Koma ngati chibamba chotuba chankala mumalo yake ndipo sichinakule, Icho ni chipsera chachilonda ndipo wansembe afunika kumuitana kuti oyela. ²⁴ Ngati nkanda inpya na munyofu wa kupya wankala wo tuluka olo chibamba choyela. ²⁵ Ndipo wansembe azaona ngati sisi pachibamba yankala yoyela, ngati yaonekela niyopitilila pa nkanda, ngati yaoneka, ndipo matenda yoyambukila changambika mukupya, ndipo wnembe afunika kumuitana iye kuti ni odesedwa. Iyo ni ntenda yo yambukila ²⁶ Koma ngati wansembe achiona ndipo aoza kuti palibe sisi yoyela pachibamba, ndipo silipansi ya nkanda koma yasilila, wansembe afunika kumuchosapo masiku seveni. ²⁷ Ndipo wansembe afunika kumuitana kuti ni odesedwa iyo ni ntenda yoyambukila. ²⁸ Ngati chibamba chankala malo mwake ndipo icho chovimba chachokela kukupsa. ndipo wansmebe afunika kumutitana kuti ni oyela, popeza palibe chilipo kuposa chpsera chakupya. ²⁹ Ngati mwamuna olo mukazi wina namatenda yoyambukila pamutu olo kalevu levu, ³⁰ Ndipo wansembe afunika kuona muntu pali ntenda yoyambukila ngati yopitilila naknda, wansembe azamuitana kuti odesedwa. Nichonyelekeza, ni ntend yoyambukila pa mutu na paka levu levu. ³¹ Ngati wansembe aona matenda yonyekeza na kuona kuti silipansi pa nkanda, ngati mulibe sisi yakuoloumo, ndipo wansmeb azachosa muntu wantendaa yonyelekeza masiku seveni. ³² Pasiku ya seveni azaona matenda ngati yoyambukila ngati mulibe sisi yoyela, ngati matenda ya oneka yasapitilila nkanda, ³³ Pamene apo afunika kuyelewa, koma pamalo yamatenda pasagelew, ndipo ansembe afunika ku muchosa uja muntu wamatenda yonyelekeza masiku seveni pamwamba. ³⁴ Pasiku ya seveni wansmebe azaona matenda kuona ngati yaleka kuyamba munkanda. Ngati yaoneka yapitilila nkanda, ndipo wansembe afunika kumuitanaoyela. mutntu afunia kuwasha vovala vake ndipo ayela. ³⁵ Koma ngati matenda yoyenelekeza yoyambuka kwambili mu nkanda pambuyo pa wansembe atakamba kuti anali oyela, ³⁶ Wansembe afunka kumuonanso. Ngati matenda yoyambuka mu nkanda, wansembe safunika kusakila sisi yayelo. Uyo ndi odesedwa. ³⁷ Koma ngati mukaonedwa ka wansembe matenda yoyeneleka yaleka na sisi yakuda yamela pa malo, ndiyr kuti matendda yapola. Ni oyela, na wansembe afunika kumuitana kuti ni oyela. ³⁸

Ngati mwamuna olo mukazi alina vibamba voyela pa nkanda, ³⁹ wansmebe azafunika kuona muntu uyo ngati vibamba vili votuba tuba, vamene chabe ivo nivimpele voyambukila pankand. Iyi ni oyela. ⁴⁰ Ngati sisi yamutnu yachoa mumutu, ali nadazi, koma ni oyela. ⁴¹ Ngati sisi yagwela kusogolo kwamutu, ngati mpumi ndiye dazi, ni oyela iye. ⁴² Koma ngati pali chilonda chotulika pa mutu wa dazi wake olo pampumi, ni ntenda yoyambukila yamene yayamba. ⁴³ Ndipo wansmebe afunika kuona ngati kuvimba kwa malo yamatenda pa mutu wa dazi olo pa mpumi niyo botuluka, monga kuoneka kwa ntenda yoyambukila pa nkanda. ⁴⁴ Ngati zilipo, ndipo alina matenda yoyambukila komanso sioyela mubusa afunika kumuitana kuti osayela chifukwa cha matenda pamutu pake. ⁴⁵ Mutnu alina matenda yoyambukila afunikila kuvala vovala vong'ambika, sisi yake ifunika kunkala yamasiku, ufunika kuphimba pamenso pake pake pamphunp na kupunada, 'Odesedwa, odesedwa.' ⁴⁶ Masiku yinse yamene azankala namatenda yoyambukila azankala oyelesedwa. chifukwa ni odsedwa namatenda yamene angayambukise, afunika kunkala eka. Afunika kunkala kunja kwa munzi. ⁴⁷ Chovala choipisiwa naubweya, nangu na chatonje olo nyula, olo cha obenji chotungu kuchokela ku tonje olo ku nyula la lineni, ⁴⁸ olo chikumba olo chili chonse chopangiwa na chikumba- ⁴⁹ Ngati muli cha greeni olo chotuluka mu chovala, chikumba, chosuka olo nsalu yotunga olo chili chonse chopangiwa nachikumba nimatenda yamene yoyambukila, ifunika lulongozewa kuli wansembe. ⁵⁰ Wansembe afunika kuona chija cintu chamatenda, afunika kuchosapo chili chonse chamatenda masiku seveni. ⁵¹ Afunika kuonanso matenda pasiku ya seveni, Ngati ntnga yayenda ku chovala olo chili chonse chotungiwa na tonje olo nyula ya lineni, olo chikopo olo chili chonse chamene chikopa chimasebenzesewa ndipo ni matenda yoipa, chija chintu ni chodesewa. ⁵² Afunika kushoka chovala, ngakale muyalo wake, olo chongiwa na tonje olo nyula ya lineni, olo chikupa olo chili chonse chopangiwa na chikumba. Chili chonse mwamene ntena yoipa ipeeka, chifukwa inga lete matenda. Icho chintu chifunika kushokeletu. ⁵³ Ngati wansembe aona chintu chija nakuona kuti matenda siyanayende ku chovala olo ku muyalo olo chotunga chatonje olo vintu vavikumba. ⁵⁴ Azaba lamulila kuwasha chintu chamene ntenda ina pezekapo, ndipo afunika kuchichosapo masiku seveni ye nangu. ⁵⁵ Wansembe azaonachintu ngat chija chintu cha ntenda cha washiwa. Ngati ntenda sichinja maonekedwe, Ingale sinayambukile, niyo desedwa. ufunika kushoka chintu chija, Ingamkale pamene ntenda yaipisa. ⁵⁶ Ngati wansmebe achiona chintu, ndipo ngati ntenda yasilila pambuyo poiwasha, ndipo afunika kunga'mba mbali yaipisiwa kuchovala olo kuchikumba olo kuchokela ku chosoka olo kuchoka kunyula ta lineni. ⁵⁷ Ngati matenda yakali kuonekela ku chovala, kapena pa soka olo kunyula yalineni olo chili chonse chopangiwa na chikumba ili kubuka. Ufunika ku shoka chija chintu namtenda. ⁵⁸ Chovala olo chili chonse cho soka olo chotunga kuchokela ku nyula ya lineni, olo chikumba, olo chili chonse chopangiwa na chikumba-ukawasha chija chintu na matenda yayenda, icho chintu chifunika ku washiwa kachibili, ndipo chiza yela. ⁵⁹ Iyi ndiye lamulo ya ntenda mu chovala cha ubweya olo lineni, olo chili choonse chosoka olo chotunga kuchokela kutonje olo nyula ya lineni, olo chikumba olo chili chonse chopangiwa na chikumba, kuti vaikambe choyela olo chakuda."

Chapter 14

¹ Yehova anakamba kuli Mose, kuti, ² "Iyi izakankala lamulo ya mutnu odwala pasiku yosambikiwa. Iye afunika kuletewa kuli wansembe. ³ Wansembe azayenda kutuluka mu munzi ukaona muntu ngati matenda yoyambukila ya nkanda yapola. ⁴ Ndipo wansembe azalamula kuti iye wamene afunika kusambikiwa afunika kutenga nyoni zibili zamoyo mutengo wamkunguza, ubweya wofila, na hissope. ⁵ Wansembe azalamulila kuti apaye nyoni imozi pamazi oyendaanyamene yali mumbiya yadoti. ⁶ Wansembe pamene apo azatenga nyoni yamoyo na mutengo wa chida, na ubweya wofila. na hissopa, ndipo azavi ika ivi vintu vonse, kufakako na nyoni yamoyo, magari ya nyoni yamene inapaiwa mumazi yoyenda. ⁷ Pamene apo wansembe azawaza manzi kali seveni pali muntu wamene afunika kusambikiwa kuchoka kumatenda, na wansembe azamuitana kuti ni oyela. Pamene apo wansembe azalekelela nyoni ya moyo muminda yoseguka. ⁸ Muntu wamene asambikiwa azawasha vovala vake, kugela sisi yake yonse, nakusamba yeka mu manzi, ndipo azayela. Pambuyo pake afunika kubwela mu munzi, koma azankala panja pa hema siku seveni. ⁹ Pasiku ya seveni afunika kugela sisi yonse ya mutu wake, afunika kugela sisi zake zonse, afunikanso kuwasha vovla vake na kuzi sambika manzi ndipo azayela. ¹⁰ Pasiku ya nambala eyiti afunika kutenga bana bamuna babili ba nkosa, na mwana umoziwa nkosa mukazi wazaka imozi alibe cilema, na batatu amugao kumo a efa ya ufa na osakaniza na mafuta monga nsembe yaufa, na muyeso umozi wamafuta. ¹¹ Wansembe wamene amusambika azaimika muntu uka wamene afunika kusambikiwa, pamozi na vintu vija, pameneo pa Yehova pa komo yaku hema yokumanilanamo. ¹² Wansembe azatenga umozi waba nkosa bamuna naku mupasa monga nsembe yo lakwila pamozi na muyeso wa mafuta; azaba baibisi benve nansembe yo baibisila pamenso ya Yehova. ¹³ Afunika aka paye ka mwana ka nkosa kamuna mu malo mwanene ba pailamo nsembe yachimo na nsembe vopseleza, mumalo ya kachisi, popeza nsembe yachimo niya wansembe, chimozi na nsembe yo lakwila chifukwa ni yoyela maningi. ¹⁴ Wansembe azatenga magzi ya nsembe yolakwa na kuika memato ya zanja yamanja yamuuntu yamene asambikiwa, pa chibombo chaku kwanja yake yamanja, na popendela pakulu pakukwendo kwake kwamanja. ¹⁵ Pamene apo wansembe azatenga mafuta namu yeso na kutila mukwanja kwake kwamanzele, ¹⁶ nakuvi ika chimbombo chake chakukwanja lamanja mu mafuta yamene yali muzanja lamanja, na kuwaza mafuta yena na chimbombo chake kali seveni pamenso ya Yehova. ¹⁷ Wansembe azaika mafuta osalila muzanja mwake mumbali ya kwayu laku zanja lamanja kwa muntu wamene kufunika kusambikiwa, panjala ya kuzanja lamanja, na nimbombo chikulu chku phazi ya kuzanja lamanja. Afunika kufaka mafuta aya pamwamba pamagazi kuchokela ku nsembe ya cholakwa. ¹⁸ kwa aya mafuta yosalila yali mu manja mwa wansembe, azayaika pamutu pa muntu wamene afunika kusambikiwa. wansembe azapangiwa chomutetezela enve pamenso ya Yehova. ¹⁹ Manje wansembe azapeleka nsembe ya chimo na nakupanga chotetezela iye wamene afunika kusambikiwa chifukwa chosayela kwake, pasogolo pake azapaya nsembe yopeleka. ²⁰ Pamene apo wansembe azapeleka nsembe yopeleka na nsembe yaunga pa guwa. Wansembe azapana chotetezela cha muntu, ndipo azankala oyela. ²¹ Koma, ngati mutnu ni osauka sanga kwanise nsembe izi, enve angatenge mwana mwamuna wankosa umozi monga nsembe ya cholakwa kubaibisiwa, kuzipangila chotetezela chake, na limozi ya mayao kumi ya efa wa ufa wosalala na mafuta monga nsembe ya ufa, na muyeso umozi wamafuta, ²² pamozi na njiba na nkunda zibili, mona wamene akwanisila kutenga; nyoni imozi izankala nsembe ya chimo na ina nsembe yopseleza. ²³ Pasiku ya nambala eiti afunika keleta kuli wansembe pakusambikiwa kwake, kukomo ya chihema chokumanilanamo, pamenso ya Yehova. ²⁴ Wansembe azatenga mwana wankosa ngati chopeleka, azatenga pamozi nayenve muyeso wa mafuta ya olivi, na azavinyamula mumwamba pamene avionesa kuli Yehova. ²⁵ Azapaya mwana wankosa pa nsembe yolakwa, enve azatenga magari yena ya nsembe yolakwa nakuyaika kosiliza kutu kwaku zanja lanja lamanja yaua wamene afunika kusambikiwa pa chimbombo cha zanja yake yamanja, na chimbombo chikulu cha phazi yake ya kuzamba lamanja. ²⁶ Pamene wansembe azatila mafuta yena muzanja yake yaku manzele, ²⁷ nakutila chimbombo chakuzanja lamanja mafuta yena yamene yali ku kwanja kwake kwamanzele kaili seveni pamenso ya Yehova. ²⁸ Wansembe azaika mafuta yena yamene yali mu kwanja kwake kwatu yaku zanja lamanja yauja wamene afunika kusambikiwa pa chimbombo chakuzanja lamanja, nacho pondela chikulu chaku phazi ili kuzanja lamanja, malo yanozi kwamene anaika magari ya nsembe ya cholakwa. ²⁹ Azaika mafuta yali mu manja mwake pa mutu yauja wamene afunika kusambikiwa, kumupanga chotetezela chake pameneso ya Yehova. ³⁰ Afunika kupeleka nkanda imozi kapena njiba ing'ono, monga mwanene muntu akwanisila kutenga- ³¹ Imozi monga nsembe ya chimo na inongu yaufa. Ndipo wansembe azapanga chotetezela chauja wamene afunika kusambikiwa pamenso ya Yehova. ³² Iyi ndiye lamulo ya muntu yamene enve muli ntenda yoyambukila ya munkanda ya wamne sakwanisa vopeleka vofunikila vaku sambikiwa kwake." ³³ Yehova anakamba kuli Mose na Aroni, kuti, ³⁴ "Mukafika mumalo ya Kanani yamene ninakupasani inkale yanu, ngati naika ntenda yamene iyambukila munyumba ya muziko

yanu,³⁵ Pamene apo mwine wanyumba afunika kubwela naku uza wansembe. Afunika kukamba kuti, muku ona kwanga muoneka monga muli ntenda munyumba yanga.³⁶ Pamene apo wansembe azalamula kuti ba chose vintu vonse vamunyumba akalibe kuyenda kuona umboni wa matenda, kuti pasankale chili chonse munyumba chamene chizadesewa. Pasogolo oake wansembe afunika kuloba kuona nyumba.³⁷ Afunika kuona ntenda kuona ngati ili mu vipupa vanyumba, na kuona ngati ioneke yobiliwila kapena yofilila maonekedwe ya pamwamba ya vipupa.³⁸ Ngati nyumba ili na ntenda, Pamene apo wansembe azachoka, munyu nakuvala chiseko cha nyumba masiku seveni.³⁹ Ngati azabwelanso pasiku ya seveni seveni na kuyi ona ngati ntenda yayambukila kuvipupa.⁴⁰ Ngati yayambukila, wansembe azalamulila kuti ba chose myala mwanene ntenda yapezeka na kuyataila mu malo yodesedwa kunja kwa muzinda.⁴¹ Azafuna vipupa vonse vamunyumba vipaliwe, ndipo afunika kutenga vintu voipisiwa vapaliwe kunja kwa muzinda nakutenga mumalo yodesedwa.⁴² Afunika kutenga myala zinangu na kuika mu malo mwamene munachoka myala zinangu, ndipo bafunika kusebenzesa dothi inangu ku maya nyumba.⁴³ Ngati matenda yabwelanso na kuyambikila munymbaa mwamene myala za chosewamo na vipupa vapaliwa na mata futi,⁴⁴ Pamene apo wansembe afunika kubwela kuona nyumba kuona ngari ntenda yayambikila, Bgati yayambukila, iyo ntenda yo'ononga na nyumba niyo desedwa.⁴⁵ Nyumba ifunka kupwanyika. Myala, maplanga, navo mata vonse munyumba vifunika kunyamula kunja kwa muzinda kumalo yodesedwa.⁴⁶ Mo ikilapo, alionse wamene aloba munyumba ntawi yamene chavaliwa azankala wodesedwa pakana mumazulo.⁴⁷ Aliyense anagona munyumba afunika kuwasha vovala vake, na alionse anadya munyumba afunika kuwasha vovala vake.⁴⁸ Ngati wansembe aloba munyumba kuona ngati ntenda yayambukila munyumba atatamata nyumba, Apo ngati ntenda yayenda, azakamba kuti iyi nyumba niyoyela.⁴⁹ Pamene apo wansembe afunika kutenga nyoni zibili kusambika nyumba, na mutengo wa chida, na ubweya wofilila, na hissopa.⁵⁰ Azapaya nyoni imozi pamozi oyenda mu mbiya.⁵¹ Azatenga mutengo wa chida, hissopa, ubweya wofiila, na nyoni yamoyo, na ku viika mu magari yanyoni yapaiwa, mumazi oyenda, na kutuila munyumba kali seveni.⁵² Azasambika nyumba na mazazi ya nyoni na manzi yoyenda, pamozi nanyoni yamoyo, na matenda wa chida, hissopa, na ubweya wofiila.⁵³ Koma azalekelela nyoni yamoyo kuyenda kutuluka muzinda kuptia kusango yoyela, Munjila iyi afunika kupanga chotetezela nyumba, ndipo izankala yoyela.⁵⁴ Ndiye lamulo ya mitundu za ntenda yoyambukila ya nkanda na vintu vamene vima leta matenda,⁵⁵ ndi yakunyaula, na ntenda, mukuvala na munyumba,⁵⁶ kuvimba, vimpele, na chibamba chotuba,⁵⁷ kuziba pamene iliyonse yamatenda aba niyo desedwa kapena niyoyela. Ndiye lamulo ya matenda yo yambukila ya nkanda na ntenda."

Chapter 15

¹ Yehova ankamba Mose na Aroni, Kuti, ² "Kamba ku bantu ba Isreali, ukambe kuli benve, ngati muntu aliyense ali natenda ouchosa manzi mutupi yake, ankale usayela. ³ Kusayela kwake ni kamba wa dwaiswa na manzi. ngale tupi yake ichosa manzi mwing ya leka, ni yosa yela. ⁴ Paliponse po gona pamene a gona pa zankala posam yela, na chilichonse chamene ankalapo chiza nkala chosa yela. ⁵ aliyense wamene agwila po gona pake afunikila ku washa zo vala zake na ku samba iye mu manzi, azankala uasyela kufikila kamaluzo. ⁶ Aliyense wamene ankala paliponse pamene muntu wamene a chosa ntenda yochosa manzi pamene enze ankala, uja muntu afunikila ku washa zovala zake naku samba iye manzi, kuchoka apo azankala usa yela kfikila kumazulo. ⁷ Aliyense wamene agwila tuoi ya mwanene achosa manzi yamatenda afunika ku washa zovala zake na kuzi sambika mu manzi, naku nkala usayela kufikila kumazulo. ⁸ Ngati muntu wamene aliniko ku chosa manzi aka tunyila mate muntu wina wamene ali oyela, pamene apo uja muntu azafunika ku washa zovala zake naukzi sambika mu manzi, kuchoka apo azankala osayela kufika kumazulo. ⁹ Chili chonse chonkalapo chamene iye wamene achosa manzi chamene ayenda chizankala chosa yela. ¹⁰ Aliyense wamene chili chonse chamene chinsli chauja muntu chiza nkala chosa yela kufikila kumazulo, anso aliyens wamene anyamula vija vintu afunikila ku washa zovala zake na kuzisambika enve manzi, aza nkala osa yela kufikila ku mazulo. ¹¹ Aliyense muntu wamene achosa manzi akagwila kaosamba manja yake na manzi afunikila ku washa zovala zake naku zisambika enve mu manzi, kuchoka apo azankala osa yela kufikila ku mazulo. ¹² Poto iliyonsee yamene omozi achosa manzi aka gwilako ifanika ku pwanyiswa, na chigubu chili chonse cha mutengo chifunikila kusukuluziwa na manzi. ¹³ Wamene al nako ku chosa manzi aka yelesewa kuzo choka, pamene apo afunika ku belenga masiku yali seveni ku yelesedwa kwake; pamene apo azafunika ku washa zovala zake naku sambika tupi yake mu manzi yo mutaika. kuchoka apo aza yelesewa. ¹⁴ Masiku yasanu na yatatu afunika ku tenga tu kunda tubili mwina tu bana twa kunda tubili naku bwela kuli Yehova pongenela mu chihema chokumanilanamo; kwaicho afunika kupasa nyoni kuli abusa. ¹⁵ Abusa afunika kupeleka, imozi pelekelo ns inangu pelekelo yoshoka, na abusa azafunika kupanga chitetezero kuli Yehova kamba kazochoka zake. ¹⁶ Ngati muntu aliyense atulula phavu yachimuna, azafunika kusamba tupi yake yonse mu ma nzi; azankala osayela kufikila kumazulo. ¹⁷ zovala zilizonse mwina chikumba funika ku washa na manzi chinkala chosa yela kufikila kumazulo. ¹⁸ Ngati mwamuna agona na mukazi kwa kala kutuluka phavu yachimuna, bonse bafunika ku samba na mnazi naku kala bosa yela kufikila kumazulo. ¹⁹ Ngati mukazi ali kumwezi, kusa yelesewa kwake ku pitiliza masiku yali seveni, kuchoka apo aliyense azankala osayela kufikila kumazulo. ²⁰ Vili vonse vame ne agonapo ntawi yaku mwazi viza nkala vosa yela; vilivonse vame ne ankalapo viza nkala vosa yel. ²¹ Aliyense wamene agwila pogona pake afunika ku washa vovala vake na kuzisambika enve eka mu manzi; uja muntu azankala osayela kufika kumazulo. ²² Aliyense wamene agwila chilichonse chamene ankalapo afunika ku washa vovala vake nakuzisambika mu manzi; uja muntu azankala osayela kufika kumazulo. ²³ inga nkale na pogona pake mwina ku chilichonse chamene ankalapo, ngati agwila, uja muntu azankala osayela kufikila kumazulo. ²⁴ Ngati muntu aliyense agona naye, ngati kusayela kwake kutikila kwamu gwila enve, azankala osayela masiku yali seveni. pamalo yamene agona paza nkala posayela. ²⁵ ngati mukazi achoka magari pali masiku yambii yamene si ntawi wake yaku mwezi. mwina ngati ku choka mwazi ku pitilila ntawi yake, mu ntawi yama siku yo tuluka yosa yela yake, azankala ngati monga ali mu masiku yaku mwezi. si oyela. ²⁶ Paliponse pamene agona mu ntawi ya chaka magari yaza nkala ngati monga po gona mumasiku ya mwezi, kuchoka apo vili vonsde vame ne ankalapo viza nkala vosa yela, monga kusa yela kwa mwezi yake. ²⁷ Aliyense wamene agwila vintu azankala osayela; afunika ku wasa vovala vake nakuzisambika mumanzi, kuchoka apo azankala osayela kufika kumazulo. ²⁸ Koma ngati ayeleswa mu kuchoka magari, kuchoka apo azazibelengela enve eka masiki yali seveni, kuchoka apo azankala oyelesewa. ²⁹ Pa siku ya namba eiti azatenga tu nkunda tubili na kutuleta kuli abusa pongenela mu chihema chokumanilamo. ³⁰ Abusa azapeleka nyoni imozi ngati sembe yachimo na inangu sembe yo shoka,, kuchoka apo azapanga yochingiliza kwaiye pamanso ya Yehova chifykwa kusa yelesewa kwake ku choka magari. ³¹ Ndiye mwamene muzaba patulila bantu ba Isreali kuchoka kusa yelesewa kwao, kwichi sibaza mwalila kamba kosa yela kwao, kamba ko'onga hema tanga, mwamene ni nkala pakati pao. ³² Aya ndiye malamulo ya aliyense wamene achoka manzi, kwa mwamuna wamene achosa phavu ya chumuna kuchoka wa enve na kumupanga osayela, kwa aliyense mukazi wamene aliku mwezi, ³³ kwa aliyense na vochoka va manzi, mwina mwamuna mwina mukazi, anso kwa mwamuna wamene agona na muzimai osayelesewa."

Chapter 16

¹ Yehova anakamba na Mose kuti-ichi chenze pamene banafa bana bamuna ba baili ba Aroni, banafa pamene banayenda nofika pafupi na Yehova. ² Yehova anakamba kuli Mose kuti, "Kamba na Aroni mubulu wako na kumu uza asazibwela pa ntawi iliyonse mu malo yoyela mukati mwa ketani, pali cholalila cha chitetezelo chapa likasa. Ngati azachita azafa. chifukwa nimonekela mu makumbi pamwamba pa chovalila chapa chitetezo. ³ Manje unu ndiye mwamene Aroni afunkila kubwela mu malo yoyeka. Afunikila kuloba na mwana wa ng'ombe chopeleka cha chimo, na mwana wa mbelele ngati chopeleka choshoka. ⁴ Afunika kuvala malaya ya nyula yoyela ndipo afunika kuvala nyula mukati mwa mukanjo pa enve eka, ndipo afunika kuvala ka nyula pasogolo na nyula yovala kumutu. Iyi ni mukanjo yoyela. Afunika kusambika tupi yakr mu manzi na kuzivalika na vovala ivi. ⁵ Afunika kutenga pa musonkano ya bantu ba Isilayeli mbuzi zimun a zibili ngait chopeleka choshokewa. ⁶ Aroni afunika kupeleka ng'ombe monga chopeleka cha chimo, chamene cha enve eka, kuzipangila chitetezelo cha enve eka na banja yake. ⁷ pamene apo afunikila kutenga mbuzi na kuzi ika pamenso pa Yehova pongenela pa hema ya yokumanilanamo. ⁸ Pamene apo Aroni afunikila kuponya vosankila va mbuzi vibili, chosankila chimozi cha Yehova, na chinangu chosankila cha mbuzi yopulumuso. ⁹ Aroni afunika kupeleka mbuzi yamene chosankila chagwela pa Yehova, na kupeleka mbuzi iyo ngati chopeleka cha chimo. ¹⁰ Koma chosankila chamne chawela pa mbuzi ya chomasulila ifunikila kuileta ya moyo kuli Yehovaa, kuti apange chotetezela paku chitumiza mu chipululu ngati chomasulila. ¹¹ Pamene Aroni afunikila kupeleka ng'ombe ya chopeleka cha chimo, chamene chizankala cha enve eka. Afunika kupanga chotetezela cha enve eka na banja yake, Afunika kupaya ng'ombe ngati cha chimo cha enve eka. ¹² Aroni afunikila kutenga mbuzi yozula na malasha ya mulilo kuchokela pa guwa ya pamenso pa Yehova, na kwanja yake kozula na voshoka va nsembe vogaya bwin, na kulea ivi vintu mukati mwa ketani, ¹³ Apo afunikila kuika vonukila pa mulilo ya pamenso pa Yehova kuti chusi chochokela ku vonunkila vizinikile chvalila pa chotetezela pamwamba pa pangano ya malamulo. Afunikila kuita ichi kuti asafe. ¹⁴ Afunikila kutenga magaz ya ng'ombe na kuyamwaza na chikumo pasogolo pa chovalila chapotetezela. Afunikila ku mwaza magari yenangu chikumo kali seveni pa chovalila chapotetezela. ¹⁵ Pamene apo afunikila kupaya mbuzi ya chopeleka cha chimo chamene chili cha bantu na kuleta magari mkati mwao ketani. Apo afunikila kuchitanayo magari monga mwamnene anachitila na magari ya ng'ombe: afunikila kuimwaza pa chovalila pa chotetezela. ¹⁶ Afunika kupanga chotetezela cha malo oyela chifukwa cha vochita voipa va bantu ba Isilayeli, na chifukwa chaku ukila kwa na machimo yabo. ¹⁷ Aliyense asankale mu hema yokumanilanamo ngai Aroni angenamo kupanga chitetezo mu malo oyela, mpaka naku choka panja ndipo asiliza kupanga chitetezo cha enve na banja yake, na cha gulu yonse ya Isilayeli. ¹⁸ Afunika kuyenda pa guwa ya pamens pa Yehova na kuipangila chitetezo, afunika kutenga magari ya ng'ombe na magari ya mbuzi na kuika pa mansego mozunguluka guwa. ¹⁹ Afunika ku mwazapo magari na kakumo kake kali seveni kuti aituvise na kuipatula kuli Yehova, kuichosa ku vochita ku bantu ba Isilayeli. ²⁰ Ngati asiliza va chitetezelo chamalo yoyela, chihema chokumanila, na guwa, afunika ku kuleta mbuzi yamoyo. ²¹ Aroni afunikila kuika manja yake pa mutu pa mbuzi ya moyo naku lapavoipa vonse va bantu ba Isilayeli, ku'ukila kwao konse namachimo yabo yonse. manje afunika kuika machimo yaja pamutu pa mbuzi na kuitumiza mbuzi manja mwa untu osamalila wamene nokukonzekela kusogolela mbuzi muchipululu. ²² Mbuzi ifunikila kunyamula voipa vonse va bantu ku malo ya eka kuja kuchipululu. mwamuna afunikila kuileka mbuzi iziyendela. ²³ Manje Aroni afunikila kubwelela mu chihema chokumanilanamo na kuvula mikanjo yamene yenze vovala akalibe kuyenda mumalo yamene yenze avala akalibe kuyenda mu malo yoyela, ndipo afunikila kusiya mikanjo pamene apo. ²⁴ Afunika kusambika tupi yake na manzi yoyela, na kuvala vovala vake na ntawi yonse; afunikila kuchoka panja na kuzishoela nsembe na kushoka nsembe ya bantu, munjila iyi apange chotetezela chake na cha bantu. ²⁵ Afunikila ku shoka mafuta ya nsembe yama chimo pa guwa. ²⁶ Mwamuna wamene anaimasula mbuzi kuti iziyendele afunika ku washa vovala vake naku sam a tupi yake na manzi; kuchokapo, angabwele futi mu munzi. ²⁷ Ng'ombe ya nsembe ya chimo na mbuzi ya nsembe ya chio, yamene magari yake yanaletewa kupanga chitetezo mu malo yoyela, ifunika kupelekewa panja pa muzi. kuja bafunikila kushoka vikumba, nyama, na matuvi. ²⁸ Mwamuna wamene azashoka ivo vintu afunikila kuwasha vovala vake na kusamba tupi na manzi; kuchoka apo, angabwele futi mu munzi. ²⁹ Limeneli ndi lamulo lanu nthawi zonse kuti, m'mwezi wachisanu ndi chiwiri, pa tsiku lakhumi la mweziwo, mudzichepetse ndi kusagwira ntchito iliyonse, kaya ndi wobadwa kapena mlendo amene akukhala pakati panu. ³⁰ Izi zili choncho chifukwa tsiku lino lidzaphimbidwa machimo anu, kukuyeretsani ku machimo anu onse kuti mukhale oyera pamaso pa Yehova. ³¹ Ili ndi Sabata lakupumula la inu, muyenera kudzichepetsa osagwira ntchito iliyonse. Limeneli ndi lamulo pakati panu nthawi zonse. ³² Mkulu wa ansembe, amene adzadzozedwe ndi kudzozedwa kuti akhale wansembe wamkulu m'malo mwa abambo ake, ³³ ayenera kupanga chotetezerachi ndi

kuvala zovala zansalu, ndiye zovala zopatulika. Aziphimba malo opatulika koposa; azichita chotetezera chihema chokumanako ndi guwa lansembe, ndipo aphimbe machimo a ansembe ndi anthu onse a mumsonkhano.³⁴ Limeneli ndi lamulo kwa inu nthawi zonse, kupepesera ana a Isiraeli machimo awo, kamodzi pa chaka. ”Izi zinachitika monga momwe Yehova analamulira Mose.

Chapter 17

¹ Yehova anakamba kuli Mose kuti, ² "kamba na Aroni na bana bake bamuna na bonse bantu baku Isireli. Bauze Yehova zamene alamullia: ³ Aliyense mwamuna apaya ng'ombe, mbelele, olo mbuzi mu msasa, olo apaila panja pamu msasa, kuti apeleke nsembe - ⁴ Ngati sazabwelesa ku chihema kokumanilana kuti apeleke nsembe kuli Yehova pasogol pa chalichi yake, uyo mwamuna alina mulandu kumucosa magari. atila magari, naye mwamuna niku mujuba pakati pa bantu bake. ⁵ Cholinga cha lamulo iye ni chifukwa bantu ba Isireli bazakazileta nsembe kuli Yehova pongenela mu chihema chokumanilanamo, kuli abusa kuti bapeleleke nsembe monga chiyanjano kuli Yehova, mumalo mopeleka mu munda oseguka. ⁶ Abusa azatila magari pa sinta ya pongenelako ku chihema chokumainlamo; azashoka mafuta kuti yachose kafungo ka bwino ka Yehova. ⁷ Bantu bazafunika kuleka kupeleka nsembbe kuli mafano ya mbuzi, wamene bachita ngati mahule. Ichi chizakala chifanizo chosaila nakuli bantu bamu mibadwo babo. ⁸ Muzakamba kuli benve, 'Mwamuna aliyense wamu Isireli, olo mulendo wamene ankala pakati panu, wamene amapeleka nsembe zo shoka olo nsembe ⁹ nosabwelesa pongenela mu chihema chokumanilamo pakuti apeleke nsembe kuli Yehova, uyo mwauna azafunika kumujuba kuli bantu bake. ¹⁰ Ngati muntu wamu nyumba ya Isireli, olo mulendo wamene ankala pakati panu adya magari, niza nkala okalipa kuli uja muntu azadya magari niza mujuba pakati pa bantu bake. ¹¹ Chifukwa umoyo wachinyama uli mu magari yake, nakupasani magari yake kuti mupange chitetezo pa guwa pali moyo wanu, chifukwa magari ndie yatetezela moyo. ¹² Chifukwa ninakamba kuli bantu bamu Isireli kuti muntu ali pakati panu asadya magari, nangu mulendo wamene ankala pakati panu kudya magari. ¹³ Aliyense muntu wanu Isireli, olo aliyense mulendo wamnene ankala pakati pabo, wamene saka naku paya nyama olo nyoni yamene inga dyeke, uja muntu azafunika kutaya magari naku ya vininkila magari na dothi. ¹⁴ Moyu wa chinyama chilichonse ni magari. ndiye chifukwa ninakamba kuli bantu baku Isireli, "Musadye magari ya chinyama chili chonse, chifukwa moyo wa chinyama ulimu magari yake. Aliyense azadya niku mujuba." ¹⁵ Aliyense wamene akudya chinyama chazifela olo chapayiwa na nyama zamu sanga, angakale ni obadwila muziko olo mulendo pakati apnu awashe vovala vake naku zisambika, azankala na doti paka kumazulo kuchoka apo azankala alibe doti. ¹⁶ Koma ngati sana washe olo kusamba pa mubili wake, ninshi anyamule mulandu wake.

Chapter 18

¹ yehova anakamba kuli, kuti, ² "Kamba na bantu baku isilayeli na kubauza, 'Ndine Yehova Mulungu wanu. ³ Simufunika kuchita vintu vamene bantu bamu Iguputo bamachita, kwamene mwenzeli kunkala kudala. Musachite vintu vamene bantu bamachita mu Kenani. Malo yamene niku pelekani. Musa konke myambo zao. ⁴ Ma weluzo yanga niyamene mufunika kuchita, ndipo malamulo yanga ndiye yamene mufunika ku sunga kuli muyendemo, chifukwa ndine Yehova Mulungu wanu. ⁵ Mwaicho mufunika ku sunga malamulo yanga. Ngati mwaya mvelela, azankala wa moyo chifukwa cha yenve. ndine Yehova. ⁶ Usafika pafupi pa mubulu wako wapafupi na kumuvula, Ine ndine Yehova. ⁷ Usavule bamai bako; niba mai bako, sufunika kuba vula. ⁸ Usa vule bakazi batate bako; nichintako chaba tate bako. ⁹ Usa vule mulondo wako, anga nkale ni mwana waba tate bako olo mwana waba mai bako, anga nkale anakulila pa nyumba panu olo kutali naimwe. ¹⁰ Usa vule mwana mukazi wa mwana wako mwamuna olo mwana mukazi, chifukwa chintako chabo ni chintako chako. ¹¹ Usa vule mwana mukazi wa bakazi baba tate bako, okulisiwa mu banja ya batate bako, chifukwa ni mulongo wako. ¹² Usa vule mulongo waba tate bako; niba bululu bako. ¹³ Usa vule mulongo waba mai bako, nibabululu baba mai bako. ¹⁴ Usa vule mubale waba tate bako, ndiye kuti, usafune mukazi wake; niba anti bako. ¹⁵ Usa vule mukazi wa mupongozi wako mukazi; ni mukazi wa mwana wako mwamun: siufunika kumu vula. ¹⁶ Usa vule mukazi wa mubale wako; ndiye kuti niwa mubale wao. ¹⁷ Usa vule mukazi na mwana wake mukazi; ndipo siufunika ku tenga mwana mukazi wa mwana olo mwana mukazi wa mwana wako mukazi kuti umu vule; niba chibululu; uku nikuyipa mutima. ¹⁸ Usa kwatile mulongo wa mukazi wao kumu panga muazi wachibili na kumuvula pamene mukazi wako akali moyo. ¹⁹ Usafike pafupi pa mukazi na kumuvula mu ntawi yamene ali kumwezi. ²⁰ Usa gone na mukazi wa muzako naku kuziyipisa na enve munjila iyi. ²¹ Siufunika kupasa aliyense pa bana bako kumu faka mumulilo, kuti uba pase nsembe kuli Moleki, chifukwa siufunika kuipisa zina ya Mulungu wako. Ine ndine Yehova. ²² Usa gone naba muna banzako monga ugoni na mukazi; ivo nivonyansa. ²³ Usa gone na chinyama chili chonse nakuziyoisa na chenve. Mukazi nayenve asazipeleke kuli chinyama naku gona nacho; iyo ni sokonezo. ²⁴ Musazi ononge mweka munila iliyonse monga izi, chifukwa mu njila zonse izi, ma ziko yamene niza chosa pamenso panu. ²⁵ Muzinda una onongeka, mwaicho ninaba langula pama chimo yabo ndipo malo yana luka benzeli kunkalapo. ²⁶ Mwaicho mufunika ku sunga mau yanga na malamulo yanga, simufunika kuchita vili vonse vonyansa ivi, ungankale obadwila mu Isilayeli olo kapena mulendo wamene ankala na imwe. ²⁷ Chifukwa ichi nichoipa chamene bantu bamu malo banachita, benzo nkala muno mukalib kubwelamo, ndipo manje malo ya onongeka. ²⁸ Mwaicho munkale bo chenjela kuti malo yassamu lukeni naimwe pambuyo pa kuyi ononga, monga mwamene ina lukila bantu benzo nkalamo mukalibe kubwelamo. ²⁹ Aliyense wamene achita ivi vintu vonyansa, bantu bamene banachita ivi vintu baza jubiwa pa bantu babo. ³⁰ Mwaicho mufunika ku sunga lamulo yanga, kosachita chili chonse pali izi myambo zo nyansa zamene zenso chitika kuno mukalibe kubwela, chakuti musazi ononge chifukwa cha venve. Ndine Yehova Mulungu wanu."

Chapter 19

¹ Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, ² Nena ndi khamu lonse la ana a Israyeli, nuti kwa iwo, Muyenera kukhala oyera, popeza Ine Yehova Mulungu wanu ndine woyera. ³ Ali wonse ayenela kulemekeza mai wake na tate wake, nafuti muyenela kusunga masabata yanga. Ine ndine Yehova Mulungu wanu, ⁴ musatembenukire kwa mafano acabe, kapena kudzipangira milungu yacabe: Ine ndine Yehova Mulungu wanu. ⁵ Mukamapereka nsembe yachiyanjano kwa Yehova, muziipereka kuti mulandiridwe. ⁶ Azizidya tsiku lomwelo popereka, kapena tsiku lotsatira. Ngati kanthu katsalira kufikira tsiku lachitatu, chiotchedwe ndi moto. ⁷ Akadyanso kanthu tsiku lachitatu, ndiyo nyama yodetsedwa; siziyenera kulandiridwa, ⁸ ndipo ali yense akachidya azikhala ndi mlandu wake, chifukwa waipsa chopatulika cha Yehova; munthuyo amchotsere anthu a mtundu wake. ⁹ Mukamakolola zokolola za minda yanu, musamakolole ngodya zonse za m'munda mwanu, kapena kututa zokolola zanu zonse. ¹⁰ Musamakunkha mphesa zonse za m'munda wanu wamphesa, kapena kutola mphesa zomwe zagwa pansi m'munda wanu wamphesa. Uzisiyira osauka ndi mlendo. Ine ndine Yehova Mulungu wanu. ¹¹ Musabe. Osanama. Osanamizirana. ¹² Usalumbire dzina langa monama, ndi kuipsa dzina la Mulungu wako. Ine ndine Yehova. ¹³ Osazunza mnzako kapena kumubera. Malipiro a wantchito sayenera kukhala nanu usiku wonse mpaka m'mawa. ¹⁴ Usatemberere wogontha, kapena kuyika chopunthwitsa pamaso pa wakhungu. Koma muziopa Mulungu wanu. Ine ndine Yehova. ¹⁵ Musapangitse chiweruzo kukhala chabodza. Musamakondere wina chifukwa ndi wosauka, ndipo musamakondere wina chifukwa ndiwofunika. M'malo mwake, weruzani mnzako molungama. ¹⁶ Usayendeyende pofalitsa miseche pakati pa anthu amtundu wako, koma tetezani moyo wa mnansi wanu. Ine ndine Yehova. ¹⁷ Usamamuda m'bale wako mumtima mwako. Uzidzudzula mnzako moonu mtima kuti ungadzichitire tchimo chifukwa cha iye. ¹⁸ Osabwezera kapena kusungira chakukhosi aliyense wa anthu ako, koma m'malo mwake konda mnansi wako monga umadzikondera wekha. Ine ndine Yehova. ¹⁹ Muzisunga malamulo anga. Osayesa kubereketsa ziweto zanu ndi mitundu ina ya nyama zina. Osakanizira mbewu ziwiri zosiyana mukamabzala m'munda mwanu. Osamavala zovala zopangidwa ndi mitundu iwiri yosakanikirana. ²⁰ Aliyense amene agona ndi mdzakazi amene walonjezedwa mwamuna, koma amene sanawomboledwe kapena kupatsidwa ufulu, ayenera kulangidwa. Sayenera kuphedwa chifukwa sanali mfulu. ²¹ Mwamuna azibweretsa nsembe yake ya kupalamula kwa Yehova pakhomu la chihema chokumanako, nkhoa yamphongo monga nsembe ya kupalamula. ²² Pamenepo wansembe aziphimba machimo + ake ndi nkhoa yamphongoyo monga nsembe yamachimo pamaso pa Yehova, chifukwa cha tchimo limene wachita. Ndiye kuti tchimo lomwe wachita lidzakhululukidwa. ²³ Mukadzafika mdzikolo ndikubzala mitengo ya mitundu yonse kuti muzidya, pamenepo muziwona zipatso zomwe amabala monga zoletsedwa kudya. Zipatso ziyenera kukhala zoletsedwa kwa inu kwa zaka zitatu. Sayenera kudyedwa. ²⁴ Koma m'chaka chachinayi zipatso zonse zidzakhala zopatulika, ndi nsembe yotamanda Yehova. ²⁵ Khumi mungadye chipatsocho, podikirira kuti mitengo ibereke zambiri. Ine ndine Yehova Mulungu wanu. ²⁶ Musadye nyama iliyonse muli magazi. Musafunse mizimu zamtsogolo, ndipo musayese kulamulira ena ndi mphamvu zamatsenga. ²⁷ Simumazungulira ngodya za mutu wanu kapena kumeta ndevu zanu. ²⁸ Osamadzicheka thupi lako chifukwa cha akufa kapena kuyika mphini pathupi lako. Ine ndine Yehova. ²⁹ Osanyozetsa mwana wanu wamkazi pomupanga kukhala hule, kuti mtunduwo ungagwere uhule ndipo dzikolo lidzadzaza ndi zoipa. ³⁰ Muzisunga masabata anga ndi kulemekeza malo opatulika a chihema changa. Ine ndine Yehova. ³¹ Osatembenukira kwa iwo amene amalankhula ndi akufa kapena ndi mizimu. Musawafunefune, kuti angakuipitseni. Ine ndine Yehova Mulungu wanu. ³² Muyenera kudzuka pamaso pa mutu wa imvi ndikulemekeza kupezeka kwa nkhalamba. Uziopa Mulungu wako. Ine ndine Yehova. ³³ Mlendo akakhala nanu m'yourdziko lanu, musam'chitire choyipa chilichonse. ³⁴ Mlendo wakugonera kwa inu mumuyese pakati pa inu monga wa m'dziko momwemo wa Israyeli, wokhala pakati panu, ndipo muzim'konda monga mudziyese nokha; popeza munali alendo m'dziko la Aigupto. Ine ndine Yehova Mulungu wanu. ³⁵ Musagwiritse ntchito njira zabodza poyesa kutalika, kulemera, kapena kuchuluka. ³⁶ Muyenera kugwiritse ntchito masikelo, miyezo yolondola, miyezo wa efa wolondola ndi hini wolungama. Ine ndine Yehova Mulungu wako, amene ndinakutulutsa m'dziko la Aigupto. ³⁷ Muzisunga malemba anga onse ndi malamulo anga onse, ndi kuwachita. Ine ndine Yehova. ”

Chapter 20

¹ Yehova anakamba kuli Mose, kuti, ² "Kamba kuli bana ba Isilayeli, 'aliyense ali pakati pa bantu ba Isilayeli, kapena mulendo aliyense wamene ankala mu Isilayeli wamene apasa bana bake kuli Moleki, afunika ka paiwa. bantu bamu malo bafunika kumu tema myala. ³ Niza mupindimukila nkope yanga muntu na kumu chosa pakati pa bantu bake chifukwa apasa mwana kuli Moleki, chakuti cho ononga malo oyela na kulakwila ina yanga yo yela. ⁴ Ngati bantu ba mumalo avala menso kuli muntu pamene apapsa mwana aliyense kuli Moleki, ngati siba mupaya, ⁵ ninshi ine neka niza pindamukila uja muntu na mubado wake, ndipo za mudolo iye ndipo aliyense wamene achita chiwelele kwa pye yehka kuchita uhule na Moleki. ⁶ Muntu wamene a pindamuka kuli bamene bakamba na bakufa, olo kapena kuli baja bamene ba kamba na mizimu kwa ichi kuchita uchiwele wele benve beka, niza mupindimukila nkope yanga uja muntu; niza mu chosapo pakati pa bantu bake. ⁷ Mwaicho sikozekeleline imwe mweka naku nkala boyela, chifukwa ndine Yehova Mulungu wanu. ⁸ Mufunikila ku sunga malamulo naku yanyamula. Ndine Yehova wamene anakupatulani imwe ngati oyela. ⁹ Aliyense wamene a tembelela ba tate bake kapena bamai bake afunika zo'ona ku paiwa, chakuti ni olakwa afunika kufa. ¹⁰ Mwamuna wamene achita chigololo namu kazi wa mwamuna winangu, chifukwa chake, aliyense wamene achita chigololo na mukazi wamukazake wa pafupi na enve-mwamuna ochita chigololo ochita chigololo bonse bafunika kupaiwa. ¹¹ Ngati mwamuna agona naba kazi baba tate bake, ninshi bavula chintako chaba tate bake. Bonse mwana mwamuna namu kazi waba tate bake bafunika ku paiwa. Magazi yabo yali pali benve. ¹² Ngati mwamuna agona na mukazi wamwana wake, bonse babili bafunika kubapaya. Benve bachita chonyansa. Bali na mulandu bayenela kufa. ¹³ Ngati mwamuna agona na mwamuna muzake, monga na muzimai, bonse ba chita chonyansa. bafunikila ku paiwa. Bali na mulandu bafunika kufa. ¹⁴ Ngati mwamuna akwatila mukazi naku kwatila na bamai ba mukazi, ichi nichoipa. Bafunikila ku shokewa, pamozi enve na bazimai, chakuti kusankale choipa pakati panu. ¹⁵ Ngati mwamuna agona na chinyama, afunikila ku paiwa, mufunika naku paya chinyama. ¹⁶ Ngati muzimai akonka chinyama naku gona nacho, muzafunika kupaya muzimai na chinyama. Muzimai na chinyama bafunika che kufa. Bali na mulandu ndipo bafunika ku paiwa. ¹⁷ Ngati mwamuna atenga kalongosi wake, mwana mukazi waba tate bake olo kapena waba mai bake, nakumuvula chintanko chake, naku ona chintako chake, ni chasone maningi. Bafunika kuba chosapo pakati pa menso yabana babo. Avununkula chintako chamu kalongosi wake, afunikila kunyamula kulakwa kwake. ¹⁸ Ngati mwamuna agona na mukazi pamene ali kumezi naku muvula chintako chake, amuvununkula kuchosa, kutaikila kwa magazi yake. Bonse mwamuna na mukazi bafunika kuba juba pakati pa bantu babo. ¹⁹ Sufunika ku vula chintako chaba kalongosi waba mai bake, olo kapena mulongosi waba tate bake, chifukwa uza chitisa nsoni ba bululu banu bapa fupi. ufunika ku nyamula kulakwa kwako. ²⁰ Ngati mwamuna agona naba kazi baba alume bake, sana chitle ulemu bamalume bake. Baza nyamula ma chimo yabo, nakufa balibe bana. ²¹ Ngati mwamuna akwatila mukazi wamu bale wake pamene mubale wake akali moyo, ni chamanyazi. Sana muchitile ulemu mubale wake, niza ba pokela bana bake makatundu yamene bana lobela kumakolo babo. ²² Muzafunika kusunga malamulo yanga navo kamba vanga; mufunikila kuya mvelela yenve chakuti mumalo yamene niku pelekankone imwe kuti isa kulukeni. ²³ Musayende mu mwamba yama ziko yamene niku choselani kuli imwe chakuti niba pishe pamenso panu, chifukwa bachita ivi vintu vonse, ndipo naba nyansa. ²⁴ Nina kamba kuli imwe kuti, "Muza landila malo yabo; Nizakupasani imwe kuti muka nkale nayo, malo yozulila na mukaka na uchi. Ine ndine Yehova Mulungu wanu, wamene anaku patulani ku bantu bena. ²⁵ Mufunikila kuvisiyanisa vinyama voyela na vosayela, na vinyonyi voyela na vosayela. Musazi ononge na vinyama vosayela na olo kapena vinyoni olo kapena chili chonse cholengewa chamene chiyenda pansi, chamene na siyanisa ngati chosa yela kuli imwe. ²⁶ Mufunikila kunkala oyela, chifukwa Ine, Yehova, ndine oyela, ndipo naku patulani imwe pa bantu bena, chifukwa ndimwe banga. ²⁷ Mwamuna olo kapena mukazi wamene akamba nabo kufa olo mizimu afunika kupaiwa. Bantu bafunikila kumutema myala. Bali na mulando bafunikila kufa."

Chapter 21

¹ Ndipo Yehova anati kwa Mose, Nena ndi ansembe, ana a Aroni, nunene nao, Munthu aliyense asadziditse pakati pa anthu a m'dziko lao, ² kupatula abale ace apafupi okha, amace, atate wace, mwana wake wamwamuna, mwana wake wamkazi, mbale wake, ³ kapena mlongo wake wa namwali amene amamdalira, popeza iye alibe mwamuna; ⁴ Asadziipitse ndi abale ake, nadzidetsa; ⁵ Ansembe asamete ndevu zao, kapena kumetera pandunji pa ndevu zao, kapena kuzimeta matupi ao. ⁶ Azikhala oyera kwa Mulungu wawo, osanyoza dzina la Mulungu wawo, chifukwa ansembewo amapereka nsembe zopsereza za Yehova, mkate wa Mulungu wawo. Chifukwa chake ansembewo ayenera kukhala oyera. ⁷ Asakwatire mkazi wachiwerewere ndi wodetsedwa, ndipo asakwatire mkazi wosiyidwa ndi mwamuna wake, chifukwa apatulikira Mulungu wawo. ⁸ Mupatulire; popeza ndiye wopereka mkate kwa Mulungu wanu; Azikhala woyera kwa inu, chifukwa Ine Yehova wakukupatulani, ndine woyera. ⁹ Mwana wamkazi aliyense wa wansembe amene adzidetsa pokhala hule amanyoza abambo ake. Iye ayenera kuti awotchedwe. ¹⁰ Iye amene ali mkulu wa ansembe pakati pa abale ake, amene adadzoza mafuta odzoza pamutu pake, ndipo wapatulidwa kuti avale zovala zapadera za mkulu wa ansembe, asamamete tsitsi lake kapena kung'amba zovala zake. ¹¹ Sayenera kupita kulikonse komwe kuli mtembo ndikudziyipitsa, ngakhale atate wake kapena amayi ake. ¹² Mkulu wa ansembe sayenera kuchoka kumalo opatulika a chihema kapena kuyipitsa malo opatulika a Mulungu wake, chifukwa wapatulidwa kukhala mkulu wa ansembe ndi mafuta odzozera a Mulungu wake. Ine ndine Yehova. ¹³ Wansembe wamkulu ayenera kukwatira namwali akhale mkazi wake. ¹⁴ Asakwatire wamasiye, mkazi wosiyidwa, kapena mkazi wachiwerewere. Sadzakwatira akazi amtunduwu. Asakwatire namwali wochokera kwa anthu a mtundu wake, ¹⁵ kuti asadetse ana ake pakati pa anthu a mtundu wake, chifukwa Ine ndine Yehova, wamene amuyelesa." ¹⁶ Pamenepo Yehova analankhula ndi Mose, nati, ¹⁷ Uza Aroni, ndi kuti, Ali yense wa ana anu m'mibadwo yawo yonse ali ndi chilema, asayandikire kukapereka kwa Mulungu wake. ¹⁸ Munthu aliyense amene ali ndi chilema asayandikire kwa Yehova, monga munthu wakhungu kapena munthu amene satha kuyenda, wolumala kapena wolumala, ¹⁹ munthu amene ali ndi dzanja lopunduka kapena phazi, ²⁰ nsana kapena wochepa thupi kapena wamfupi modabwitsa, kapena mwamuna wopunduka m'maso mwake, kapena wodwala matenda, zilonda, nkhanambo, kapena amene machende ake aphwanyidwa. ²¹ Munthu aliyense mwa ana a Aroni wansembe wopanda chilema asayandikire kukapereka nsembe zotentha ndi moto za Yehova. Munthu wotero ali ndi chilema; asayandikire kuti apereke chakudya cha Mulungu wake. ²² Akadye chakudya cha Mulungu wake, kaya ndi zopatulika koposa kapena zina zopatulika. ²³ Asalowe mkatikati mwa katani kapena kubwera pafupi ndi guwa lansembe, chifukwa ali ndi chilema, kuti angaipitse malo anga opatulika, chifukwa ine ndine Yehova amene ndimawapatula. ²⁴ "Pamenepo Mose analankhula mawu amenewa. Aroni, ana ake, ndi anthu onse a Israeli.

Chapter 22

¹ Yehova anakamba na Mose, Nati, ² Kamba na Aroni na kubana bake bake bamuna, bauze kuti bankale patali ba vintu ku vintu vopatulika va banthu ba Israele, zamene bamanipatulila ine. Basaipise zina langa loyela. Ine ndine Yehova. ³ Kamba nao, "ngati kuli aliyense wa mbeu zanu zonse mumibandwe ofika pafupi ku vintu vopatulika vamene banthu ba Israele bapatulila Yehova, panene ali osayela, uyo munthu afunika kujubidya pasogolo panga. Ine ndine Yehova. ⁴ Kulibe mbeu ya Aroni ali na khate, kapena matenda yochokela mu tupi, azadya nsembe yopangidwa ya Yehova kufikila akankala oyela. Aliyense azagwila chilichonse chosayela kupitila mu kukumana na bakufa, olo kapena kukumana na mwamuna wamene achosa mpavu zaumuna, ⁵ olo aliyense azangwila nyama yokalaba yamene imupanga kunkala osayela, kapena munthu wamene amulengesa kunkala osayela, ngankale chilichonse chosayela. ⁶ Ndipo opeleka nsembe azagwila chosa yela azankala osa yela kufikila mumazulo. Safunika kudya chintu chili chonse choyela, koma ngati asamba tupi yake mumanzi. ⁷ Koma zuba ikangena, azankala oyela. Pambuyo pake zuba ikangena angadye ku vintu voyela, chifukwa nivake vakudya. ⁸ Asadye chili chose chamene azapeka chakufa, kapena chopaiwa na nyama zamusanga, mwaichi angazioneke eka. Ndine Yehova. ⁹ Opeleka nsembe afunika kukonka malangizo, chifukwa bazapezeka na chimo ndipo bangafe pakuniipisa ine. Ine ndine Yehova wamene nibapanga boyela. ¹⁰ Kulibe aliyense wa kunja kwa banja ya opeleka nsembe, kufakilako naba lendo ba opeleke ba nsembe kapena wolembedya nchito, bangadye chili chonse chopatulika. ¹¹ Koma wansembe akagula kapolo na ndalama zake, uja kapolo angadye ku vintu vopatulika kwa Yehova. Ba banja wa wansembe naba kapolo bana badwila mu nyumba yake, nawo bangadye naye vintu ivo. ¹² Ngati mwana mukazi wa ansembe akwatiliwa to muntu wamene sali wansembe, asadyeko vopatulika va chakumi chamusonko. ¹³ Koma mwana wamukazi wa ansembe akankala wofedwa, ochosedwa ku chikwati, kapena alibe mwana, ndipo akabwelela kunkala kunyumba kwa ba tate bake monga anali wachichepele, angadye vakudya va batate bake. Koma kulibe wina wamene sali mubanja mwa ansembe wamene angadye vakudya vaba nsembe. ¹⁴ Ngati muntu adya chakudya chopatulika mosaziba, afunikila kulipila kwa ansembe pachakudya chamene icho; afunika kufakilapo wanu-fithi nakubwezanso kwa ansembe. ¹⁵ Banthu ba Israele sibafunika kuipisa vintu vopatulika vamene bafaka pamwamba na kupeleka kwa Yehova, ¹⁶ ndi kulengesa iwo kunyamula uchimo wamene uzabapanga kuchimwila vakudya vopatukila, Ine ndine Yehova wamene amakuyelesani." ¹⁷ Yehova akamba na Mose, kuti, ¹⁸ "Kamba na Aroni na bana bake bamuna, na kubanthe bonse ba Israele. Bauze kuti, "Alibonse mu Israele, kapenga mulendo onkala mu Israele, akabwelesa nsembe, kapena nikukwanilisa chipangano, kapena nichopasa cha kuzifunila, kapena babwelesa kwa Yehova chopeleka cha nsembe, ¹⁹ ngati chifunika kulandilidwa, bafunika kupasa nyama imuna yamene ilibe ulema kuchokela ku ng'ombe, nkhoa kapena mbuzi. ²⁰ Koma simufunika kupasa chilichonse chili na ulema. Sinizachivomela mumalo mwanu. ²¹ Wamene apasa sembe yoku sonkana chopeleka kuchokela ku ng'ombe kapena nkhoa twa Yehova kukwanilisa chipangano, kapena kupasa mwamene afunila, sichifunika kunkala cholemala kuti chilandilidwe. Simufunika kunkala Ulema mu nyama. ²² Musapase nyama yosaona, yoduka mendo, kapena yopunduka, kapena yafundo, yavilonda na yoonongeka. Simufunika kupeleka vaso kwa Yehova monga nsembe ya mulilo pa guwa yansembe. ²³ mungabwelese monga chopasa chabe monga ng'ombe kapena nkhoa yamene inakula kapena ing'ono, chifukwa monga icho sichizalandilidwa mu chipangano. ²⁴ Osapasa nyama kwa Yehova yamene ili yozichita, yopwanyika, yoonongeka kapena yojubika ziwalo. Osachita ichi mumalo yanu. ²⁵ Musazilangiza buledi ya Mulungu mu manja ya ma folena. Izo nyama nizovunda ndiponso nizolemala, sizizalandilidwa kwa imwe. ²⁶ Yehova anakamba na Mose kuti, ²⁷ "Koma ng'ombe kapena nkhoa kapena bunzi ikabadwa, ifunika kunkhala masiku yali seveni na bamai baker. Kuyambila pasiku la namba eiti, ingalandilidwe monga nsembe pa chopasidwa kwa Yehova. ²⁸ Osapaya ng'ombe kapena nkhoa, pamozi na mwana, vonse pasiku imozi. ²⁹ Mukapasa chopeleka choyamika kwa Yehova, mupeleke munjila mwamene ifunikila. ³⁰ Ifunika kudya usiku wamene uyo yalandilidwa monga sembe. Osasiyako kalikonse kufikila mailo. Ine ndine Yehova. ³¹ Koma mufunika kusunga malamulo yanga na kuyachita. ³² Musaipise zina yanga loyela. Muzindikile kuti ndine oyela naku banthu ba Israele. Ndine Yehova woku yelesani. ³³ Wamene anakuchosani ku ziko ya Ejipito kunkala Mulungu wanu; Ndine Yehova."

Chapter 23

¹ Yehova anakamba na Mose kuti: ² Kamba na bantu ba Isilayeli, ukamba nabo kuti, 'Ivi ndiye zoika zikandwelelo za Yehova, vamene mufunika kulalikila ngati bosonkana boyela pamozi; ivi nivikondwelelo vanga ntawi zonse. ³ Munga sebenze pamasiku yali, koma siku ya 7 ni Sabata yopumula, kusunkana koyela. Musachite nchito ili yonse chifukwa ni Sabata ya Yheova mumalo monse mwamene munkala. ⁴ Ivi ndiye voikika vikondwelelo va Yehova, musonkano oyela wamene ufunika ku ulusa ntaei zoikika. ⁵ Mumwezi oyamba, pasiku ya fotini mu mwezi kumazulo, ni pasika Yehova. ⁶ Pa siku ya fifitini mu mwezi umozi ni chikondwelelo chamukate ulibe chofufumisi ya Yehova pakuti masiku yali 7 ufunika ndiye mukate ulibe chofufumisa. ⁷ Siku yoyamba uyi patule kukumana pamozi; Suzachita nchito zili zonse zamene umachita. ⁸ Uzapeleka chakudya chopeleka kuli Yehova pama siku yali 7. Siku ya Sabata ni musonkano wopatulika wa Yehova, ndipo pa siku iyo musachite nchito yamene mumachita ntawi zonse.' ⁹ Yehova anakamba na Mose, Kutu, ¹⁰ "Kamba na bantu ba Isilayeli naku bauza kuti, 'pamene muzabwela muziko yamene niza kupasani, napamene muzachosa zamene muzakolola, maje mufunika kuleta mpukusu ya vipaso voyamba va mbeu kuwa nsembe. ¹¹ Azanyamula mpukusu ya mbeu pamenso pa Yehova naku zipeleka kuli iye kuti zivomelezewe mu malo yanu. Nipa siku pamene Sabata yapita pamene wansembe azanyamula naku chibwelelesa kuli ine. ¹² Pasiku yamene muzanyamula mpukusu ya mbeu naku leta kuli ine, mufunikila kuleta kankosa ka chaka chimozi kamene kalibe choipa chilichonse ngati nsembe yopyeleza ya Yehova. ¹³ Mbeu zopeleka zifunika kuknkala zibili za teni za efa ya flaulo yopepuka yosakaniza na mafuta chopeleka chopangiwa na mafuta, chopeleka chopangiwa na mulilo kuli Yehova, ina chakumwa chopela cha vinyu, na folo ya wini. ¹⁴ Simufunika kudya mukate, kapena vakudya voyocha mbeu zo-oneka bwino, kufikila siku yamene imozi yamene uzaleta chopelea kuli Mulungu wako. Ichi chizankala chilamulo chanuyaya kumibadwo yabantu bako bonse na mumalo yonse yamene muzankala. ¹⁵ Siku yoyamba Sabata itapita-ndiye siku yamene munaleta ma mpukusu ya mbeu ngati chopeleka chonesa mumwamba-belengani ma Sabata yatatu yokwanila. ¹⁶ Mufunika mubelenge masiku yali fiftite, yamene yafunika kunkala siku itapita Sabata. Manje ufunika kupasa chopeleka cha mbeu yasopano kuli Yehova. ¹⁷ Mufunuika kuleta mukate ubili kuchokela mumanyumba yanu wopangiwa kuchokela mu zibili za teni ya efa. yafunika kupangiwa kuchokela mu flaulo yopepuka naku pika na chotupisila; Vizankala chopeleka cho-oneso mumwamba chavipaso voyamba kuli Yehova. ¹⁸ Ufunika kupeleka mukate na nkosa bali 7 kunkala nsembe yopyeleza kuli Yehova, na mbeu zake zopeleka na chakumwa chake chopeleka, chopeleka chopangiwa na mulilo naku chosa kafungo konukila kabwino kwa Yehova. ¹⁹ Ufunika kupeleka mbuzi imozi imuna pachopeleka chauchimo, na nkosa zibili zachaka chimozi za nsembe, ngatu chopeleka chamusonkano. ²⁰ Wansembe afunka kuvionesa kumwamba vonse pamozi namu muakate wa vipaso voyamba pamenso ya Yehova, naku vipasa kuli iye ngati chopeleka nankpsa zibili. Vizankala vopeleka voyela kuli Yehova vaba nsembe. ²¹ Uzafunika kupanga chi uluso pa siku imozi yamene ija. Kuzankala kusunkana koyela, musachite nchito yachabe. Iyi izankala lamulo paka muyaya kumibadwo yabantu bako bonse namumalo yonse yamene muzakankala. ²² Pamene mwachosa zokolola zamu ziko yanu, simufunika kuchosa mu makomo yonse yamu munda, mfunika ku unjika vosala mu munda mwakukolola kwanu. Mufunika kusiyako vabovutika nabaku ziko yachilendo. Ndine Yehova Mulugnu wanu.'" ²³ Yehova anakamba na Mose, anati, ²⁴ "Kamba na bantu ba Isilayeli naku bauza mumwezi wa 7, siku yoyamba yamwezi ya kuzankala kupimula opanda vochit, kukumbukila naku liza kwalipenga, namusonkano oyela. ²⁵ Usachite nchito yachabe, ufunika kupeleka nsembe yopangiwa na mulilo kuli Yehova.'" ²⁶ Ndipo Yehova anakamba na Mose, anati, ²⁷ "Manje siku ya teni yamu mwezi muna wa 7 nisiku ya chitettzo. Ifunika kunkala musonkano oyela, mufunika kuzichepesa naku kupeleka kuli Yehova chopeleka na mulilo. ²⁸ Musachite nchito iliyonse pa siku iyo chifukwa ni siku ya chitetezo, kuzipangila chitetezo paimwe mweka pamaso ya yehova Mulungu wanu. ²⁹ Aliyense wamene sazichepesa pa siku iyo afunika kuchosewa ku bantu bake. ³⁰ Aliyense wamene achita nchito iliyonse wamene achita nchito iliyonse pa siku iyo, Ine, Yehova, niza muononga kuchokela pakati pa banru bake. ³¹ Sufunika kuchita nchito ya mutundu uli onse pa siku ija. Ichi chizankala chilamulo paka muyaya kumi badwo yabantu bako bonse namuamlo yonse yamene muzankalamo. ³² Siku iyi ifunika kunkala kuli iwe Sabata yopumula mopanda vochachita mufunikila kuzichepesa pa siku ya 9 ya mumwezi kumazulo kuchoka kumazulo kufika kumazulo mufunika kukonka Sabata." ³³ Yehova anakamba na Mose, anati, ³⁴ "Kamba na bantu ba Isilayeli, kuti, 'pasiku ya sisitini yamu mwezi wa 7 kuzankala chikondwelelo chamutunzi wa Yehova. Chizankala ma Siku 7. ³⁵ Pa siku yoyamba kuzankala ku sanku na koyela. Musachite nchito ya chabe. ³⁶ Mumasiku yalu 7 mufunika kupeleka nsembe yopangiwa pa mulilo kul yehva, Pa sikuya 8 kufunika kunkala musonkano oyela, ndipo mufunika kupanga kupeleka nsembe yapa mulilo kuli Yehova. uyu nimusonkano ulibe vochitika, simufunika kuchita nchito ilioyonse ya chabe. ³⁷ Ivi ndiye vikondwelelo voikikika va Yehova, vamene mufunika ku lalikila ngati musonkano yoyela kupeleka nsembe

pa mulilo kuli Yehova, mbeu, nsembe na vinyu vopeleka chilionse pa siku yake.³⁸ Ivi vikondwelelo vizankala vo onjezela ku masabata ya Yehova na mpaso yanu, kulumbika wnu kwaise, nazopeleka mofulumiziwa imwe mweka zamene mupasa kuli Yehova.³⁹ kulingana na chikandwelelo chamu mitunzi, pasiku ya 15 mu mwezi wa 7, pamene mwaika pamozi muvipaso vamu malo, mufunika kusunga ichi chikondwelelo cha Yehova pama siku 7. Kopanda chochiti na siku ya 8 nayo kuzankala kupumula kopanda chochita.⁴⁰ Pasiku yoyamba ufunika kutenga vipaso vabwino maningi kuchokela ku mutengo, misambo yaka njeza, yogundila, na misondozo yaku manzi, ndipo muzakondwela pamanso pa Yehova Mulungu wanu pama siku 7.⁴¹ Pama siku 7 chaka chili chonse, mufunika kusekelela chikondwelelo ichi kuli Yehova. Ici chizankala chilamulo paka muyaya kumibadwo yabantu bako bonse namumalo yonse yamene muzaka nkalamo. Mufunika kusekelela chiondwelelo ichi mu mwezi wa 7.⁴² Mufunuika kunkala mutumakumbi tungono pamasiku 7. Bonse bamene bana badwaila mu isilayeli bafunika kunkala mutumakumbi tungonopamasiku 7,⁴³ kuti bodwa muli iwe, mibadwo kuchokela-mibadwo, banga punzile mwamene niapangila bantu ba Isialyeli kuti bankale mutumakumbi tungono pamene ninaba sogolela muziko ya Iguputo. Ndine Yehova Mulugnu wanu."⁴⁴ Muli iyi njila, Mose ana ulusa kuli bantu ba isilayeli pa zoikika zikondwelelo za Yehova.

Chapter 24

¹ Yehova anakamba kuli Mose, kuti, ² "Lamulila bantu ba Isilayeli ku leta mafuta yoyela yo chosewa ku mpesa yo sebenzesa mu nyali, kuti nyali ku nga yake mosa leka. ³ Kunja kwa ketani yamalamulilo yachipangano mu tenti mo kumanilana, Aroni afunika ku salekeza, ku choka usiku mpaka ku seni, sunga nyali pa menso ya Yehova inkale yo yaka. Ichi cho umba chiza nkala chamuyayaya cho yondelela mbadu wa bantu bako. ⁴ Wa nsembe mukulu afunika ku yasha nyali ntawi zonse pa mensi ya Yehova, nyali paika nyali golide yoyela. ⁵ Mufunika ku tenga flaulo yo salala naku kazingila mukate ili twelofu. Pafunika ku nkala gawo yabili ya efano tenths mukate ili yonse. ⁶ Pamene apo mufunika kupangamo mu vokonkamo vibili, navo konkamu mu mzela, pa table ya golide yo yela pa sogolo pa Yehova. ⁷ Mufunika ku faka ku nunkila kwa bwino ko yelo mu muzela mukate monga nsembe yoyimililako. uku ko nunikila kwa bwino ku zankala ku shokela Yehova. ⁸ Pa Sabata ili yonse ba nsembe ba pambwa bafunikila ku panga mukate pa sogolo pa Yehova ku mbali kwa bantu ba Isilayeli, monga chipangano chamuyayaya. ⁹ Iyi nsembe izi nkala ya Aroni na bana bake ba muna, ndipo bazadyela pa malo poyela, nichifukwa ni chi gawo cha nsembe kuli Yehova chopangika na mulilo." ¹⁰ Manje vina chitika ku mwana wa mukazi waku Isilayeli, bamene batate bake banali baku Iguputo, bana yenda pakoti pa bantu ba Isilayeli. ¹¹ Uyu mwana mwamuna waba Isilayeli mukazi bana menyana na mwamuna wa isilayeli mu musonkano. Mwana mwamuna wa mukazi waku Isilayel ananyoza zina ya Yehova naku mutembelela Mulungu, chakuti bantu bana muleta kuli Mose zina yaba mai bake inali Shelomiti, mwana wa Dibri, ku chokela mu mutundu wa Dani. ¹² Bana mu gwila nakumu manga mpaka Yehova eka sfunika ku kamba chi funilo chake kuli benve. ¹³ Pamene Yehova anakamba kuli Mose, kuti, ¹⁴ "Tenga mwamuna wamene atembelela Mulungu panja pa musonkano. Bonse munvela baike manja yabo pa mutu wake, na bonse bo sonkana bamu teme myala. ¹⁵ Ufunika kuba londolela bantu bamu Isilayeli naku kamba, aliyense wamene atembelela Mulungu aza nyamula mu landu wake. ¹⁶ Aliyense wamene anyoza zina ya Yehova afunikila ku paiwa. Bonse bo kumana bafunika kumu tema myala, anga nkale mlendo olo obadwila mu Isilayeli. Ngati aliyense anyoza zina ya Yehova, afunika ku paiwa. ¹⁷ Ngati muntu aliyense achita ngozi muntu afunikila ku paiwa. ¹⁸ Ngati aliyense achita ngozi chinyama cha muntu wina, afunika kumu bwezela umoyo pa umoyo. ¹⁹ Ngati muntu aliyense achiga ngozi kuli munzake, chifunika kuchita kuli enve vamene achitila munzake: ²⁰ ngozi pa ngozi, menso pa menso, meno pa meno. mwamene achitila ngozi kuli muntu, ndipo chi nkale nso chochitiwa kuli enve. ²¹ Aliyense wamene apaya nyama afunika kulipila, na mutnu aliyense apaya muntu afunika ku paiwa. ²² Mufunika kunkala na lamulo imozi bonse ba bili mulendo na obadwila mu Isilayeli, chifukwa ndine Yehova Mulungu wanu." ²³ Chakuti Mose anakamba kuli bantu ba Isilayeli, ndipo bantu banaleta mwamuna panja pa musonkano, wamene anatembelela Yehova. Bana mutema na myala. Bantu ba Isilayeli bana tenga lamulo ya Yehova kuli Mose.

Chapter 25

¹ Yehova anakamba kuli Mose pa lupili ya Sinayi, kuti, ² "Kamba na bana ba Isilayeli na kubauza, 'Mukabwela muziko ya mene nakupasani ziko iyo ifunika kusunga Sabata kwa Yehova. ³ Mufunika kubyala munda wako zaka sikisi, kwazaka sikisi ufunika kudula munda mwako ilaku kolola chipaso. ⁴ Koma chaka cha namba seveni, Sabata yopumula ya ziko ifunika kulemekezewa, Sabata ya Yehova. Usabyala munda wako kapena kudula mu munda. ⁵ Usakolola vozikulila veka, osakolola mpesa zokula kuli mipesa yosadulidwa munda. Ichi chiza nkala chaka chopula cha Yehova muziko. ⁶ Vilivonse vomela mumunda osalimiwa muziko mu chaka cha Sabata ziza nkala zakudya zanu. iwe, banchito bako na balendo bamene ba nkala na imwe banga tenge vokudya, ⁷ na vibeto vako na nyama zamu sanga zingadye vamene nkaka ibala. ⁸ Ufunika kubelenga masabata seveni, yamene ni kali seveni kuchulukisalapo zaka seveni, kti kuknkale masabata seveni ya zaka, kukwanila zaka fote naini. ⁹ Pamene apo ufunika kulinza lipenga kuli konse pa siku yateni ya mwezi wa seveni. Pasiku la chitetezo ufunia kuliza lipenga muziko lonse. ¹⁰ Ufunika kupatula chaka cha fifite kwa Yehova naku kambazaulu muziko lonse kuli bantu bonkalamo. Izi nkala ni jubili kwa imwe, mwamene katundu na bakapolo afunika kubwezewa kuma banja yabo. ¹¹ Chaka cha fifite chizankala cha jubili kwa imwe,. Osasunga kapena kukolola. Idyani vili vonse vozimelela, kololani mpsea zamene zimela muminda yo sauidwa. ¹² Popeza ni jubili yamene izankala yoyela kwaiwe ufunikakudya vipasa vamene vikula veka kunja kwa minda. ¹³ Ufunika kubweza aliyense ku vintu vake mu chaka cha jubili. ¹⁴ Ngati wagulisa malo yako kuli ba neba bako kapena wagula malo kuli neba wako, osanamami kapena kuchita choipa. ¹⁵ Ngati wagula malo kuli neba wako, belenga nambala ya zaka na mbue zamene zinga kololewe paka jubili inangu. Neba wako wamene agulisa malo afunika kuona nayenve. ¹⁶ Nambala ya zaka zambili paka jubili yamene ibwela izachulukisa mutengo ya malo, nambala ing'ono yazaka paka jubili yamene ibwela iza chepesa mtengo, chifukwa namba ya vokolola malo yazabala ya mwini wake ili ngana na namba ya zaka zapa mbuyo pa jubili ina. ¹⁷ Osanama kapena kuyambana na aliomse; koma ufunika kulemeka Mulungu, popeza ndine Yehova Mulungu wako. ¹⁸ Chifukwa chake ufunika kumvelela malembo yanga, sunga malamulo yanga, na kuyachita ndipo uzankala muziko bwino. ¹⁹ Ziko lizabala vipaso, uzadya naku kuta na kunkalamo bwino. ²⁰ Ukoa kukamba kuti, "Tizadya chani muntawi ya chaka cha seveni? Ona, sitinga shange kapena kukolola vipaso. ²¹ Nizalamulila daliso yanga kubwela pali iwe mu chaka cha sikisi ndipo izabala vipasa vokwanila zaka zitatu. ²² Ushanngi mu chaka cha eyiti na kupitiliza kudya kuchokela kuzaka zakumbuyo zobala na chakudya chosungiwa. paka kukolola kwa chaka cha naini kubwelanso, muzdya kuchokela muli vosungiwa na mu chaka chapa mbuyo. ²³ Malo ya gulisiwe kuli mwine wake wasopano, chifukwa malo niyanga. Mose ndimwe balendo bonkalako chabe mumalo yanga. ²⁴ Mufunika kuvomereza chilolezo chakuombol cha malo ya gulisiwa kuli banjan kwamene unagulako. ²⁵ Ngati mbale wako wamu Isilayeli wasaika na chifukwa chaicho anagulisa chintu chake, mubale wake wapafupi afunika kubwela na kuombola vamene mubale wake agulisa. ²⁶ Ngati muntu alibe mubale wake bo bombola chintu chake, koma ngati ayenda pasogolo ndipo alinayo mpavu yo chiombola, ²⁷ pamene apo ayike zaka pamozi kuchokela ntawi yamene malo yana gulisiwa nakulipila ndalama yo salako kuli muntu kwamene anagulisa pamene apo akoza kubwelelela kumalo yake. ²⁸ Koma ngati sakwanisa kutenganso malo yake ya enve, ndipo malo yamene anagulisa izasalila mumanja yauja anaigula paka chake cha jubili. pa chkae cha jubili, malo ya zabwezewa kuli muntu anaigulisa, na mwine wake wamene azabwelele kuchintu chake. ²⁹ Ngati muntu agulisa nyumba mu muzinda walinga, ndipo angai gulenso mu chaka itagulisiwa. kwa chaka chimozi azankala na mpavu yo'ombola. ³⁰ Ngati nyumba sina ombolewe muchaka chija, ndipo nyumba ili mu muzinda wozunguluka izankala katundu ya ogula na bana bake yachikalile. sichifunika kubwezewa muchaka cha jubili. ³¹ Koma manyumba ya mumenzi yalibe vzunguluka azakala monga ya muziko. Yakoza kuombolewa, yafunika kubwezewa muntu ya jubili. ³² Koma, manyumba ya alevi mumizinda yao yanga ombolewe ntawi iliyonse. ³³ Ngati umozi mwa Levi saombla nyumba anagulisa, ndipo nyumba yamene ina gulisiwa mu muzinda mwamne inali ifunika kubwezewa muchaka cha jubili, popeza manyumba ya alevi ni katundu yabo pakati kabana ba Isilayeli. ³⁴ Koma minda yozunguluka mizinda zao sizingagulisiwe chifukwa ni malo ya alevi ni malo ya alevi yachikalile. ³⁵ Ngati muntu muzako wamuziko ankale osauka, chakuti sakwanisa kuzisunga, mufufinka kumu tandiza monga munga mungatandizile mulendo kapena alionse okala ngati waukunja pakati kaimwe. ³⁶ Osamulipilisa ndalama ya pamwamba kapena phindu kuchka kwaiye munila iliyonse, koma lemekeza Mulungu wako kuti mubale wako apitilize kunkala naiwe. ³⁷ Osamubweleka ndalama na kumulipilisa ya pamwamba, kapena kumugulisa vakudya kuti upeze phindu. ³⁸ Ndine Yehova Mulungu wako, wamene anakutulusa muziko ya Iguputo, kuti nikupase malo ya kanani, nikuti ninkale Mulungu wako. ³⁹ Ngati mbale wanu wamuziko ankal osauka na kuzigulisa kuli iwe, osamusebenzese monga kapolo wako. ⁴⁰ Musunge mona ni olembewa nchito, Afunia ku nkala monga muntu wamene ankala naimwe ka ntawi kan'ono.

Azakutumikila naiwe paka chaka cha jubili. ⁴¹ Pamene azachoka kuli iwe, Iye nabana bake, ndipo azabwelela ku banja lake naku katundu yaba tate bake. ⁴² Chifukwa niba nchito banga bamene nintulusa muziko la Iguputo. Sibazaguliswa munga bakapolo. ⁴³ Osabalamulile iwo moba nzunza, koma ufunika kumekeza Mulungu. ⁴⁴ Koma kuli akapolo bakazi na bamuna, bamene ungapeze kuma ziko yo nkala pafupi naimwe, ungagule akapolo kuli benve. ⁴⁵ Ungagulenso akapo kuli balendo bamene bankala pakati paimwe na kuchokela ku banja yabo yamene bali naimwe, bamene banabadwila muziko mwanu, kuti bankale katundu yanu. ⁴⁶ Ungapeleka akapolo aba munga choloba cha bana bako pambuyo pako, kusunga munga katundu nakuba panga ukapolo moyo wabo bonse, koma musama sogolela abalebani pakati kabana ba Isilayeli mu ba nzuna. ⁴⁷ Ngati mulendo kapena muntu wamene ankala naimwe kantawi kan'olo ankala olemela, ngati umozi wa Isilayeli anakla osauka na kuzigulisa kuli mulendo uja, kapena ku mutnu wa banja ya mulendo, ⁴⁸ ngati mubale wanu wa Isilayeli aguliwa, akoza kuguliwa futi wina mu banja yake anga muombole. ⁴⁹ Angankale ndi amalume ba uja muntu, kapena mwana wa bamalume bake, bamene amuombola, kapena aliyense ali mubanja mwake, kapena angankale wandalama, angazi ombole yeka. ⁵⁰ Afunika kubelenga pamozi na muntu anamugula, afunika kupenda zaka kuchokela ntawi anazigulisa yeka kuliomugula paka chaka cha jubili. ⁵¹ Ngati pakali zaka zambili kufika chaka cha jubili, afunika kulipila mona mutengo wa maomboledwe yake ya muyeso wandalama olingana zaka zija. ⁵² Ngati kwasala zaka zing'ono kufika chaka cha jubili, afunika kupenda na omugula kuti baone namba ya zaka zapasogolo jubili ikalibe kufika, ndipo afunka kulipila maomboledwe yake mukusunga na manamba yazaka. ⁵³ Afunika kumutenga munga mwamuna olembewa nchito chaka na chaka. ⁵⁴ Ufunika kuonesha kuti sasungiwa monzunziwa. Ngati sana bombolwe na njila izi, afunika asebenze paka jubili yenve na bana bake. ⁵⁵ Kwaine bana ba Isilayeli ni banchito. Ni banchito banga bamene ninatulusa muziko ya Iguputo. Ndine Yehova Mulungu wako.

Chapter 26

mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo.⁴¹ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, munga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Shelumieli mwana mwamuna Zurishaddai.⁴² Pa siku ya nambala sikisi, Eliasaph mwana mwamuna wa Deuel, musogoleli wa mubadwe wa Gad, anapasa chopeleka chake.⁴³ Chopeleka chake chinali mbale imozi ya siliva yolema 130 mashekele na mbale imozi ya siliva yolema sevente mashekele, kulingana na kulema kwa mumalo yo yela. Ivi vintu vibili venze vozula na fulaulo yopepuka yosankanizikana na mafuta na mafuta ya nsembe ya mbeu.⁴⁴ Anapasa futi mbale imozi ya golide yolema teni mashekele, yozula vonunkilisa.⁴⁵ Anapasa munga nsembe yo shoka bulu umozi, mbele imozi, na ya chaka chimozi - chobadwa -mbelele imuna.⁴⁶ Anapasa mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo.⁴⁷ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, munga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Eliasaph mwana mwamuna Deuel.⁴⁸ Pa siku ya nambala seveni, Elishama mwana mwamuna wa Ammihud, musogoleli wa mubadwe wa Ephraim, anapasa chopeleka chake.⁴⁹ Chopeleka chake chinali mbale imozi ya siliva yolema 130 mashekele na mbale imozi ya siliva yolema sevente mashekele, kulingana na kulema kwa mumalo yo yela. Ivi vintu vibili venze vozula na fulaulo yopepuka yosankanizikana na mafuta na mafuta ya nsembe ya mbeu.⁵⁰ Anapasa futi mbale imozi ya golide yolema teni mashekele, yozula vonunkilisa.⁵¹ Anapasa munga nsembe yo shoka bulu umozi, mbele imozi, na ya chaka chimozi - chobadwa -mbelele imuna.⁵² Anapasa mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo.⁵³ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, munga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Elishama mwana mwamuna Ammihud.⁵⁴ Pa siku ya nambala eiti, Gamaliel mwana mwamuna wa Pedahzu, musogoleli wa mubadwe wa Manasseh, anapasa chopeleka chake.⁵⁵ Chopeleka chake chinali mbale imozi ya siliva yolema 130 mashekele na mbale imozi ya siliva yolema sevente mashekele, kulingana na kulema kwa mumalo yo yela. Ivi vintu vibili venze vozula na fulaulo yopepuka yosankanizikana na mafuta na mafuta ya nsembe ya mbeu.⁵⁶ Anapasa futi mbale imozi ya golide yolema teni mashekele, yozula vonunkilisa.⁵⁷ Anapasa munga nsembe yo shoka bulu umozi, mbele imozi, na ya chaka chimozi - chobadwa -mbelele imuna.⁵⁸ Anapasa mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo.⁵⁹ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, munga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Gamaliel mwana mwamuna Pedahzur.⁶⁰ Pa siku ya nambala naini, Abidan mwana mwamuna wa Gideoni, musogoleli wa mubadwe wa Benjamini, anapasa chopeleka chake.⁶¹ Chopeleka chake chinali mbale imozi ya siliva yolema 130 mashekele na mbale imozi ya siliva yolema sevente mashekele, kulingana na kulema kwa mumalo yo yela. Ivi vintu vibili venze vozula na fulaulo yopepuka yosankanizikana na mafuta na mafuta ya nsembe ya mbeu.⁶² Anapasa futi mbale imozi ya golide yolema teni mashekele, yozula vonunkilisa.⁶³ Anapasa munga nsembe yo shoka bulu umozi, mbele imozi, na ya chaka chimozi - chobadwa -mbelele imuna.⁶⁴ Anapasa mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo.⁶⁵ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, munga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Abidan mwana mwamuna Gideoni.⁶⁶ Pa siku ya nambala teni, Ahiezer mwana mwamuna wa Ammishaddai, musogoleli wa mubadwe wa Dani, anapasa chopeleka chake.⁶⁷ Chopeleka chake chinali mbale imozi ya siliva yolema 130 mashekele na mbale imozi ya siliva yolema sevente mashekele, kulingana na kulema kwa mumalo yo yela. Ivi vintu vibili venze vozula na fulaulo yopepuka yosankanizikana na mafuta na mafuta ya nsembe ya mbeu.⁶⁸ Anapasa futi mbale imozi ya golide yolema teni mashekele, yozula vonunkilisa.⁶⁹ Anapasa munga nsembe yo shoka bulu umozi, mbele imozi, na ya chaka chimozi - chobadwa -mbelele imuna.⁷⁰ Anapasa mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo.⁷¹ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, munga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Ahiezer mwana mwamuna Ammishaddai.⁷² Pa siku ya nambala leveni, Pagiel mwana mwamuna wa Okrani, musogoleli wa mubadwe wa Dani, anapasa chopeleka chake.⁷³ Chopeleka chake chinali mbale imozi ya siliva yolema 130 mashekele na mbale imozi ya siliva yolema sevente mashekele, kulingana na kulema kwa mumalo yo yela. Ivi vintu vibili venze vozula na fulaulo yopepuka yosankanizikana na mafuta na mafuta ya nsembe ya mbeu.⁷⁴ Anapasa futi mbale imozi ya golide yolema teni mashekele, yozula vonunkilisa.⁷⁵ Anapasa munga nsembe yo shoka bulu umozi, mbele imozi, na ya chaka chimozi - chobadwa -mbelele imuna.⁷⁶ Anapasa mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo.⁷⁷ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, munga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Pagiel mwana mwamuna Okrani.⁷⁸ Pa siku ya nambala tveovu, Ahira mwana mwamuna wa Enani, musogoleli wa mubadwe wa Naphtali, anapasa chopeleka chake.⁷⁹ Chopeleka chake chinali mbale imozi ya siliva yolema 130 mashekele na mbale imozi ya siliva yolema sevente mashekele, kulingana na kulema kwa mumalo yo yela. Ivi vintu vibili venze vozula na fulaulo yopepuka yosankanizikana na mafuta na mafuta ya

nsembe ya mbeu.⁸⁰ Anapasa futi mbale imozi ya golide yolema teni mashekele, yozula vonunkilisa⁸¹ Anapasa monga nsembe yo shoka bulu umozi, mbele imozi, na ya chaka chimozi - chobadwa -mbelele imuna.⁸² Anapasa mbuzi imuna imozi monga nsembe ya chimo.⁸³ Anapasa ngombe zibili, faivi mbelele, mbuzi zili faivi zimuna, na faivi mbelele zimuna zamene zinali na chaka chimozi chobadwa, monga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Iyi inali chopeleka cha Ahira mwana mwamuna Enani.⁸⁴ Basogoleli ba israeli bana patula vonse ivi pa siku yamene Mose anazozu guwa. Bana yelesa mbale zili tveovu za siliva, mbale zili tveovu zina za siliva, na mbale zili tveovu zinangu za golide.⁸⁵ Mbale iliyonse ya siliva yenze kulema 130 mashekele nainangu inali kulema sevente mashekele. Zonse mbale za siliva zinali kulema 2,400 mashekele, kulingana na chipimo chamu malo yoyela ya mashekele.⁸⁶ Iliyonse pa mbale zili tveovu za golide , zozula na vonunkilisa, zinali kulema teni mashekele kulingana na chipimo chamu malo yoyela ya mashekele Zonse mbale za golide zinali kulema 120 mashekele.⁸⁷ Bana patula zonse nyama za nsembe yoshoka, mabulu yali tveovu, mbelele tveovu, na tveovu mbelele za chaka - chimozi chobadwa. Bana pasa nsembe ya mbeu yao. Banapasa mbuzi zili tveovu zimuna monga nsembe ya chimo.⁸⁸ Kuchokela kungombe zao zonse, bana pasa yali twente - folo mabulu, sikisite mbelele, mbuzi zimuna zili sikisite, na sikisite mbelele zimuna zili na chaka chimozi chobadwa, monga chopeleka cha nsembe ya chiyanjano. Ivi vinali vo nkazikisila guwa pamene inazozewa.⁸⁹ Pamene Mose anayenda mu hema yokumanilamo ku kamba na Yehova, ananvela liu yake ikamba kuli eve. Yehova anakamba kuli eve kuchokela ku mwamba chitetezelo chovininkila pa chombo cha umboni, pakati pa ma cherabim. anakamba.

Chapter 8

¹ Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ² " Kamba kuli Aroni. kamaba kuli eve, ' Nyali zili seveni zifunika kuyakisa pa sogolo pachokilapo nyali pamene mwayasha." ³ Aroni anachita ivi. Anayasha nyali pa voikilapo nyali kuti kuoneke kusogolo, monga mwamene Yehova anauzila Mose. ⁴ Poikila nyali pana pangiwa monga mwamene umo Yehova anamulangzila Mose mwamene pafunika ku nkali. Panali kufunika ku nkala golide yokokomela kuchokela pansa kufikila kumwamba, na makapu yo kokomela monga ma fulawazi. ⁵ Nafuti, Yehova anakamba kuli Mose, Anakamba, ⁶ " tenga ba levi kuchokela pa bantu israeli nakuba yelesa. ⁷ Chita ichi kuli beve kuba yelesa: bawaze tumanzi twa chitetzelo kuli beve. Bafunika kugela tupi yao yonse, nakuwasha vovala vao, nakuziyelesa. ⁸ Ndipo leka batenge bulu mwana na nsembe ya mbeu ya fulaulo yopepuka yosankaniza na mafuta. Batenge bulu mwana wina monga nsembe ya chimo. ⁹ Uzabaleta ba levi pa sogolo pa hema yokumanilamo na kusunikanisa gulu yonse ya bantu ba israeli. ¹⁰ Pamene waleta ba levi pamenso pa Yehova, bantu ba israeli bafunika kuika manja yao pa ba levi. ¹¹ Aroni afunika kupasa ba levi pamenso pa Yehova, monga nsembe yopitisa pasogolo kuchokela ku bantu ba israeli kuti banga chite nchito ya Yehova. ¹² Ba levi bafunika kuika manja yao pamutu pa mabulu. Mufunika kupasa bulu umozi monga nsembe ya chimo na winangu bulu mnga nsembe yo shoka kuli ine, kuteteza ba levi. ¹³ Peleka ba levi kuli Aron na pamenso pa bana bake bamuna, banyamule monga nsembe yopitisa pasogolo kuli ine. ¹⁴ Mwaichi ufunika kupatula ba levi kuchoka kubantu ba israeli. Ba levi baza nkala banga. ¹⁵ Pambuyo pa icho, ba levi ba funika ku ngena mukati kusebenza mu hema yokumanilanamo. Ufunika kuba yelesa. Ufunika kubapasa monga nsembe yopitisa pa sogolo. ¹⁶ Chita ichi, chifukwa nibanga kuchokela pa bantu ba israeli. Bazatenga malo ya mwana aliyense mwamuna wamene asecula mimba, obadwa oyamba pa bonse ba mubadwe wa israeli. Natenga ba levi kunkala banga nemwine. ¹⁷ Bonse pa bobadwa boyamba kuchokela pa bantu ba israeli nibanga, pamozi bantu na nyama. Pa siku yamene ninapaya bonse bo badwa boyamba mu malo ya iguputo, ninaba si ilila kubapatula kuli ine neka. ¹⁸ Natenga ba levi kuchokela pa bantu ba israeli mumalo mwa bobadwa bo yamba bonse. ¹⁹ Napasa ba levi monga mpaso kuli Aron na bana bake bamuna. Nabatenga kuchokela pa bantu ba israeli kugwila nchito ya bantu ba israeli mu hema yokumanilanamo. Nabapasa kuteteza bantu ba israeli kuti kulibe chilango chingaba gwele bantu pamene babwela pafupi na malo yo yela." ²⁰ Mose, Aroni, na gulu yonse yabantu ba israeli bana chita ichi na ba levi. Bana chita vonse vamene Yehova analamula Mose kamba kaba levi. Bantu ba israeli bana chita ichi na beve. ²¹ Ba levi bana ziyelesa na ku washa vovala vao, na Aroni anabapeleka monga nsembe yopitisa pa sogolo kuli Yehova naku panga chitetezo chao choba yelesa. ²² Pambuyo pa icho, ba levi banangena mukati kuchita nchito mu hema yokumanilanamo pamenso pa Aroni na pamenso pa bana ba Aroni bamuna. Ichi chinali monga mwamene Yehova analamula Mose pali ba levi. Bana chita chimozi mozi kuba levi bonse. ²³ Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ²⁴ " Vonse ivi niva ba levi bali na zaka zo badwa twente faivi na kuikilapo. Bafunika kunkala mu yo sebenza mu hema yokumanilanamo. ²⁵ Bafunika ku siya ku sebenza ngati bakwanisa zaka fifite zobadwa. Pa musinku uyo bafunika kusiya kusebenza. ²⁶ Bafunika kutandiza ba bale bao bamene bapitiliza kusebenza mu hema yokumanilanamo, koma sibafunika kusebenza futi. Ufunika ku uza ba levi mu nkani zonse izi."

Chapter 9

¹ Yehova anakamba na Mose mu chipululu cha Sinai, mu mwenzi oyamba wa chaka chachibili pumbuyo po choka mu malo ya iguputo. Anakamba, "² leka bantu ba israeli pa sunge pasika pa ntau yake mu chaka. ³ Pa siku ya nambala fotini ya mu mwenzi uno, usiku, mufunika kusunga pasika pa ntau mu chaka. Mufunika ku isunga, konkani vokonka vochita, na kunvelela yonse ma lamulo yolingana nayo. ⁴ Mwaicho, Mose anauza bantu ba israeli kuti bafunika kusunga pwando ya pasika. ⁵ Mwaicho banasunga pasika mu mwenzi oyamba, pa siku yanambala fotini ya mu mwenzi, usiku, mu chipululu cha sinai. Bantu ba israeli bana nvela vonse vamene Yehova analamula Mose kuchita. ⁶ Kunali bamuna benangu bamene bana nkala bo sayela chifukwa cha tupi ya muntu wakufa. Sibanasunge pasika pa siku ija. Banayenda kuli Mose na Aroni pa siku yamene ija. ⁷ Baja bamuna banakamba kuli Mose, " sitili bo yela chifukwa cha tupi ya muntu wakufa. Nichani mutilesa kupeleka nsembe kuli Yehova pa ntau yamene inaikiwa mu chaka ba bantu ba israeli?" ⁸ Mose anakamba kuli beve, " embekezani ninvele vamene Yehova azani uza pali imwe." ⁹ Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ¹⁰ " kamba ku bantu ba israeli. kamba, ' ngati aliyense pali imwe olo mubadwe si uli oyela chifukwa cha tupi yakufa, olo n ali pa ulendo utali, anga sunge pasika kuli Yehova.' ¹¹ Mu mwenzi wachibili pa siku ya nambala fotini usiku, bazadya chakudya cha pasika. Bafunika kudya mbelele ya pasika na mukate opangiwa kuli vo fufumisa na mizyu yolula. ¹² Sibafunika kusiyo mpaka mailo kuseni, olo kutyola mabonzo yake yali yonse. Bafunika kukonka malamulo yonse ya pasika. ¹³ Koma muntu aliyense wamene si oyela ndipo sali na pa ulendo, koma akangiwa kusunga pasika, uyo muntu afunika ku chosewa kubantu bake chifukwa sanapeleke nsembe yamene Yehova afuna pa ntau inaikiwa mu chaka. Uyo mwamuna afunika kunyamula chimo yake. ¹⁴ Ngati mulendo ankala na imwe ndipo asunga pasika kuli Yehova, afunika ku isunga kulingana na malamulo ya pasika na kulingana na lamulo yake. Mufunika ku nkala na lamulo imozi ya bonse babili mulendo na wamene anabadwila mu malo." ¹⁵ Pa siku yamene kachisi inapangiwa, kumbu invininkila kachisi, hema ya chipangano cha lamulo. Usiku kumbu inali pamwamba pa kachisi. Inali kuoneka monga mulilo mpaka kuseni. ¹⁶ Inapitiliza sochabe. Kumbi inavininkila kachisi na kuoneka monga mulilo usiku. ¹⁷ Ntau zonse ngati kumbi yachosewapo pamwamba pa hema, bantu ba israeli banali kuyambako pa ulendo wao. Pali ponse ngati kumbi ya imilila, banu ba israeli banali ku panga musonkano. ¹⁸ Pa lamula ya Yehova, bantu ba israeli banali kuyenda, na pa lamulo yake, banali kusunkana. Pamene kumbi ikaimilila pamwamba pa kachisi, banali ku nkala mu musonkano. ¹⁹ Ngati kumbi ya nkala pa kachisi masiku yambili, mwaicho bantu ba israeli banali kunvelela vamene Yehova azabauza na kusayenda. ²⁰ Ntau zina kumbi inankala masiku yan'gono pa kachisi. Ngati ku monga umo, banali kunvelela lamulo ya Yehova - banali kusunkana na kuyenda futi ngati alamulila. ²¹ Ntau zina kumbi inali kupezeka mu musonkano kuchokela usiku mpaka kuseni. Ngati kumbi yanyamuka kuseni, banali kuyenda. Ngati yapitiliza muzuba na usiku, koma chabe ngati kumbi yanyamuka ndiye pamene banali kuyenda. ²² Olo ngati kumbi yankala pa kachisi masiku yabili, mwenzi umozi, olo chaka chimozi, ngati ikali pamene paja, bantu ba israeli banali kunkala pa musonkano wao nakusayenda. Koma ngati kombi yanyamuka, banali kuyambapo pa ulendo wao. ²³ Banali kupanga musonkano pa lamulo ya Yehova. Bana nvelela lamulo ya Yehova inapasiwa kuli Mose.

Chapter 10

¹ Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ² " panga malupenga yabili ya siliva. Kokomela kuyapanga. Ufunika kuyasebenzesa kuitanilako musonkano pamozi na kuitanilako musonkano kubwelela mu magulu yao. ³ Ba nsembe bafunika kuliza malupenga kuitanilako bonse ba mu musonkano pamozi pasogolo pako pa komo ya hema yokumanilanamo. ⁴ Ngati bansembe baliza chabe kamozi lupenga, mwaicho basogoleli, boyanganila mitundu ya israeli, bafunika kusonkana kuli iwe. ⁵ Ngati mwaliza mwampavu monga chozibilako, musonkano ku mbali yaku maba ufunika kuyamba ulendo. ⁶ Ngati mwaliza mwampamvu chozibilako ntau yachibili, musonkano ku mbali yaku mpoto ufunika kuyamba ulendo. Bafunika kuliza mwa mpamvu chizibilako ulendo wao. ⁷ Pamene musonkano waunjikana pamozi, lizani malupenga, koma osati mwa mpamvu. ⁸ Bana bamuna ba Aron, ba nsembe, bafunika kuliza malupenga. Ichi chizankala cho konka kuli imwe ntau zonse za mubadwe wa bantu banu. ⁹ Ngati mwa enda ku nkondo mu malo yanu na badani banu bamene bama kuvutisani, mwaicho ,ufunika kuliza chozibilako na malupenga. Ine, Yehova mulungu wanu, niza ku ganizani na kuku pulumusani ku ba dani banu. ¹⁰ Futi, na pa ntau yachisangalalo, kuika pamozi mapwando yanu ya ntau zonse na poyamba pa mwenzi, mufunika kuliza malupenga pa nsembe yanu yoshoka napa vopeleka vanu va nsembe yanu yachiyanjano. Ivi viza nkala monga chokumbukilako chanu kuli ine, mulungu wanu. Ndine Yehova mulungu wanu. " ¹¹ Muchaka chachibili, mu mwenzi wachibili, pa siku ya nambala twente ya mu mwenzi, kumbi inanyamuliwa kuchoka pa kachisi yachipangano chalamulo. ¹² Bantu ba israeli banayambapo pa ulendo wao muchipululu cha Sinai. Kumbi inaimilila mu chipululu cha Parani. ¹³ Bana panga ulendo wao oyamba, mu kukonka lamulo ya Yehova inapasiwa kuli Mose. ¹⁴ Musonkano unali pa chikwangwani cha mubadwe wa Yuda unayambilila keyenda, kuyendesha aliyense basilikali bao. Nahshoni mwana mwamuna wa Amminadabu anasogolela basilikali ba Yuda. ¹⁵ Nathaneli mwana mwamuna wa Zuar anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe Issachar. ¹⁶ Eliabu mwana mwamuna wa Helon anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe Zebuluni. ¹⁷ Mubadwe wa Gershoni na wa Mareri, banali kusunga kachisi, bana mangusula kachisi na kuyambapo ulendo wao. ¹⁸ Bokonkapo, asilikali ba chikwangwani cha musonkano wa Reubeni bana yambapo pa ulendo wao. Elizur mwana mwamuna wa Shedueri anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe wa Simeoni. ¹⁹ Shelumieli mwana mwamuna wa Zurishaddai anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe wa Simeoni. ²⁰ Eliasafu mwana mwamuna wa Deuel anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe wa Gad. ²¹ Ba Kohate banayambapo, bana nyamula vosebenzesa vamu malo yoyela. Benangu banali ku panga kachisi pamene bakalibe kufika ba Kohate pa musonkano wachibili. ²² Basilikali bapa chikwangwani cha mubadwe wa Efulemu banayambapo mokonkapo. Elishama mwana mwamuna wa Ammihub anasogolela basilikali ba Efulemu. ²³ Gamalieli mwana mwamuna wa Pedahzuri anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe wa Manasse. ²⁴ Abidani mwana mwamuna wa Gideoni anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe wa Benjamini. ²⁵ Basilikali bana sonkana pa chikwangwani cha mubadwe wa Dani banayambapo mosilizila. Ahiezi mwana mwamuna wa Ammishaddai anasogolela basilikali ba Dan. ²⁶ Pagieli mwana mwamuna wa Okrani anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe wa Asha. ²⁷ Ahira mwana mwamuna wa Enani anasogolela basilikali ba mutundu wa mubadwe wa Nafutali. ²⁸ Ndiye mwamene basilikali ba bantu ba israeli banali kuyendela pa ulendo wao. ²⁹ Mose anakamba kuli Hobab mwana mwamuna wa Reuel waku midiani. Reuel anali tate wa mukazi wa Mose. Mose anakamba kuli Hobab nakukamba, " tiyenda kumalo yamene Yehova anakamba. Yehova anakamba, ' niza kupasani.'bwelani kuli ife ndipo tizakusugani mushe. Yehova alonjeza kuchitila vabwino kuli israeli. " ³⁰ Koma Habab anakamba kuli Mose, " siniza enda naimwe. niza yenda kumalo kwanga na kubantu banga. " ³¹ Mwaicho Mose anayanka, " chonde usati siye. Uziba mo sonkanila muchipululu. Ufunika kuti londa. ³² Ngati wa enda naife, tizakuchitila vabwino monga vamene Yehova amachita kuli Mose. " ³³ Bana yenda kuchokela ku lupili ya Yehova mu masiku yatatu. Bokosi ya chipangano cha Yehova inayenda musogolo mwao mu masiku yatatu na ku peza malo yao yopumulilamo. ³⁴ Kumbi ya Yehova inali pali beve muzuba pamene banali kuyenda. ³⁵ Ntau zonse pamene bokosi ya chipangano inali chosewa, Mose anali kunena, " imani Yehova. Mwazani badani banu. Lekani abo bemene bakuzondani ba tabe kuchoka kuli imwe. " ³⁶ Ntau zonse pamene bokosi yachipangano ika imilila. Mose anali kukamba, " bwelelani, Yehova, kuli israeli zikwi zambili."

Chapter 11

¹ Manje bantu bana dandaula chifukwa chama vuto yao apo ninshi Yehova anvela. Yehova ananvela bantu ndipo anakwiya. Mulilo kuchokela kuli Yehova unashokapo bena naku shoka bamene banali mumbali mwamusonkano. ² Mwaicho bantu bana itana Mose, Mwaicho Mose anapempela kuli Yehova, na mulilo unaleka. ³ Malo yaja bana yaitana Taberah, chifukwa mulilo wa mulungu unashokapo bena pali beve. ⁴ Bena mwabantu balendo banayamba kusonkana pamozi na bamubadwe wa israeli. Banali kufuna vakudya vabwino. Mwaicho bantu ba israeli banayamba kulila nakukamba, " nibandani bazatipasa nyama yakudya? ⁵ Tikumbukila nsomba zamene tinali kudya mwaulele ku Iguputo, makukumba, ma meloni, latesi na anyezi, na galiki. ⁶ Chilakolako chakudya tilibe, chifukwa vamene tiona ni iyi mana chabe." ⁷ Mana inali monga mbeu za mpesa. Inali kuoneka monga mutengo wa njale. ⁸ Bantu banali kuyenda yenda nakuyola. Banali kui gaya muvogailamo, kutwa mu mabende, kubilisa mu mapoto, naku panga mikate. Inali kunveka monga mafuta ya mpesa yosayuma. ⁹ Ngati mame yagwela pamusonkano usiku, mana nayo inali kugwa. ¹⁰ Mose ananvela bantu badandaula mu mabanja yao, na mwamuna aliyense anali pa komo ya hema yake. Yehova anakwiya maningi, nakudandaula kwao sikunali bwino pa menso pa Mose. ¹¹ Mose anakamba kuli Yehova, " nichani mwachitila choipa kuli wanchito wanu? nichani simunakondwele naine? mwanileka kunyamula mutolo wa aba bantu bonse. ¹² Nanga ndine ninaba bala bantu bonse aba? Nanga ndine ninaba bala kuti mukambe kuli ine, ' banyamule pafupi nachifuba chako monga tate amanyamula mwana? ' Ndine nifunika kubanyamula ku malo yamene munalumbila kuli makolo yao kubapasa? ¹³ Nanga nizaizepa kuti nyama yopasa bantu bonse aba? Balila pasogolo panga nakukamba, ' tipase nyama tidye.' ¹⁴ Siningakwanise bonse aba bantu neka. Bani pakila. ¹⁵ Chifukwa mwanichitila munjila iyi, nipayeni manje - ngati napeza ubwino pa menso panu -musanivomeleze ku ona kuipa kwanga.." ¹⁶ Yehova anakamba kuli Mose, " Niletele bakulu bakulu ba israeli bali sevente. Simikiza kuti nibakulu bakulu na basilikali ba bantu. Babwelesa ku hema yokumanilanamo baimilile kuja naiwe. ¹⁷ Nizabwela kukamba naiwe kuja. Nizatenga zina mwamizimu zamene zili pali iwe na zi ika pali beve. Bazanyamula mutolo wa bantu pamozi naiwe. Si uzafunika kunyamula weka. ¹⁸ Kamba kubantu, ' ziyeeleseni mweka, chifukwa mailo kweni kweni muzadya nyama, chifukwa mwalila na Yehova anvelani. Muna kamba, " ni ndani azatipasa nyama kuti tidye? chinali bwino kwaife mu Iguputo." Mwaicho Yehova azakupasani nyama, ndipo muzazidya. ¹⁹ Simuzadya nyama siku imozi chabe, masiku yabili, masiku faivi, masiku teni, olo masiku twente, ²⁰ koma muzadya nyama mwenzi onse mpata zichokele mu mpuno zanu. Zizaku tinkani chifukwa mwakana Yehova, wamene ali pakati panu. Munalila pamenso pake. Munakamba, "Nichifukwa chani tinasiya Iguputo?" ²¹ Mwaicho Mose anakamba, " Nili na 600, 000 bantu, ndipo wakamba, ' nizabapasa nyama zokudya mwenzi onse.' ²² Tifunika kupaya mbuzi na mbelele kuti bakutile? " tifunika kugwila nsomba zonse mu manzi kuti bakutile?" ²³ Yehova anakamba kuli Mose, " kwanja yanga nanga ni ifupi? manje uzaona ngati kuti olo kapena mau yanga na ya zooni." ²⁴ Mose anachoka panja naku uza bantu mau ya Yehova. Anasonkanisa sevene bakulu pa bantu nakubaika mozunguluka hema. ²⁵ Yehova anaseluka mu kumbi nakukamba na Mose. Yehova anatengako muzimu unali pali Mose naku ika pa bakulu bakulu bali sevente. Pamene muzimu unankala pali beve, bana nenela, koma nipamene paja chabe osati nafuti. ²⁶ Bamuna babili banasala mu musonkano, mazina yao Eldad na Medad. Muzimu unabankala nabeve. Mazina yao yanalembewa, koma sibanayende panja pa hema. Olo kunachitka ivi, bana nenela mumusonkano. ²⁷ Munyamata mumusonkano anatamanga naku uza Mose, ..Eldad na Medad banenela mumu sonkano." ²⁸ Yoshua mwana mwamuna wa Nun, mutandizi wa Mose, umozi muli bamuna bamene anasanka, anakamba kuli Mose, "Mfumu yanga Mose, baimike." ²⁹ Mose anakamba kuli eve, " uninvelela kaduka kamba ka ine? Ningafune kuti bonse bantu ba Yehova bankala baneneli na kuti anagaike muzimu wake pali beve bonse!" ³⁰ Mwaicho Mose na bakulu bakulu ba israeli banabwelela mu musonkano. ³¹ Mwaicho mpepo kuchoka kuli Yehova naku bwelelsa tunyoni kuchoka pa manzi. Tunagwela pa fupi na musonkano, monga ulendo wasiku imozi kumbali imozi na ulendo wasiku imozi kumbali inangu. Tunyoni tunazunguluka musonkano ma kiyubiki yabili kuchoka pansi kuyenda mumwamba. ³² Bantu banali bontangwanika kudoba tunyoni siku yonse , usiku onse, na siku yokonkapo. Kulibe anadoba tun'gono twamene situfika votengelamo teni va tunyoni. Banagabana tunyoni musonkano onse. ³³ Nyama zikali pakati pamenso yao, pamene banali bakali kuisheta, Yehova anabakwi ila. Anabagwesela matenda yakulu. ³⁴ Malo yaja banayapasa zina Kibrothi Hattaavah, chifukwa kuja banashika bantu bamene banali nay nyama yolakalaka. ³⁵ kuchokela Kibrothi Hattaavah bantu banayenda ku Hazerathi, kwamene bana nkala.

Chapter 12

¹ Mwaicho Mirriam na Aron banakamba moshushana na Mose chifukwa cha mukazi waku shute wamene anakwatila. ² Bana kamba, " Nanga Yehova amakamba chabe na Mose? nanga sanakambe naife? Koma Yehova ananvela vamene banakamba. ³ Manje mwamuna Mose anali ozichepesa, ozichepesa kuhila aliyense pa ziko. ⁴ Pamene apo Yehova anakamba na Mose, Aron na Mirriam: " chokani panja, imwe batatu, pa hema yokumanilanamo." Mwaicho batatu banachoka panja. ⁵ Mwaicho Yehova anabwela pansu mukumbi. Anaimilila pa koma pa hema yokumanilanamo nakuiana Aron na Mirriam. Bonse babili bana bwela pa sogolo. ⁶ Yehova anakamba, " manje nvelani mau yanga. Ngati muneneli wanga ali na imwe, nizazi onesa kuli eve menso mpenya naku kamba naye mu maloto. ⁷ Wa nchito wanga Mose sali monga ivo. Ali okulupilika mu nyumba yanga yonse. ⁸ Nima kamba na Mose menso mpenya, osati mu zo onekela mu menso olo mummyambi. Amaona vilengedwe vanga. nanga nichani simuyopa kukamba moshushana naye wa nchito wanga, moshushana na Mose?" ⁹ Ukali wa Yehova unagwela pali beve, mwaicho anachokapo nakubasiya. ¹⁰ Kumbi inaimi kuchoka pa hema, na Mirriam anankala na makate - anankala otuba monga matalala. Pamene Aron anayangana kuli Mirriam, anaona kuti anali na makate. ¹¹ Aron anakamba kuli Mose, " Oh, bwana wanga, musa sungile iyi chimo kuli ife. Tinakamba mopusa, ndipo tachimwa. ¹² Chonde musamuleka kuti ankale monga obadwa manje okufa wamene nkanda yake niyokupya pamene achoka mu mimba." ¹³ Mose anaitana Yehova. Anakamba, " chonde mupoleseni, mulungu, napapata." ¹⁴ Yehova anakamba kuli Mose, " ngati atate bake bamutunyila pamenso, azankala osakondwelesa kwa masiku seveni. Muvalileni kunja kwa musonkano masiku seveni. Pakapita ivo mu mubweze futi mukati." ¹⁵ Mwaicho Mirriam bana muvalila panja pa musonkano masiku seveni. Bantu sibana yenda mpaka pamene anabwellela mu musonkano. ¹⁶ Pambuyo pa ivo, bantu banayenda kuchokela ku Hazereth nakupanaga musonkano muchipululu cha Paran

Chapter 13

¹ Mwaicho Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ² " tuma bena pali ba muna kuti bakaone malo ya k,anaani, yamene napasa bantu ba israeli. Tuma mwamuna kuchokela kumutundu onse wa makolo yake. Mwamuna aliyense afunka ku nkala musogoleli pali beve." ³ Mose anabatuma kuchokela muchipululu cha Parani, mwaicho kuti banga nvelele lamulo ya Yehova. Bonse banali ba sogoleli pa bantu ba israeli. ⁴ Aya ndiye yanali mazina yao: kuchokela ku mutundu wa Reuben, Shammua mwana mwamuna wa Zackuri; ⁵ Kuchokela ku mutundu wa Simeoni, Shaphati mwana mwamuna wa Hori; ⁶ Kuchokela ku mutundu wa Yuda, Kalebua mwana mwamuna wa Jephunneh; ⁷ Kuchokela ku mutundu wa Issachari, Igal mwana mwamuna wa Yosefe; ⁸ Kuchokela ku mutundu wa Efulemu, Hoshea mwana mwamuna wa Nani; ⁹ Kuchokela ku mutundu wa Benjamini, Palti mwana mwamuna wa Raphu; ¹⁰ Kuchokela ku mutundu wa Zebuluni, Gaddieli mwana mwamuna wa Sodi; ¹¹ Kuchokela ku mutundu wa Yosefe(uko ndiye kunena kuti, Kuchokela ku mutundu wa Manasseh), Gaddi mwana mwamuna wa Susi; ¹² Kuchokela ku mutundu wa Dan, Ammieli mwana mwamuna wa Gemalli; ¹³ Kuchokela ku mutundu wa Asher, Sethur mwana mwamuna wa Michael; ¹⁴ Kuchokela ku mutundu wa Nafutali, Nahbi mwana mwamuna wa Vophsi; ¹⁵ Kuchokela ku mutundu wa Gad, Geuel mwana mwamuna wa Maki. ¹⁶ Aya yanali mazina ya bamuna bamene Mose anatumia kuyenda kuona malo. Mose anaitana Hshea mwana mwamuna wa Nani zina yake Yoshua. ¹⁷ Mose anabatuma kuti bakaone ziko ya Kenani. Anabauza kuti, "Muyendele kuyambila ku Negevi mukayende konse mpaka kufika mu ziko ya pili. ¹⁸ Mukailangane ziko kuona mwamene ionekela. Onani bantu bamene bankalamo, ngati nibampavu kapena nibofoka, nafuti kuti kapena nibang'ono kapena nibambili. ¹⁹ Onani ziko mwamene ilili mwamene bankala. Niyabwino kapena niyoipa? Nanga muli mizinda zabwanji? Yali monga mahema, kapena ni mizinda zochingiliziwa? ²⁰ Onani na mwamene ilili ntaka, kapena kuti niyabwino kushangamo mbeu kapena iyayi, kapena kuti muli mitengo olo mulibe. Nkalani bolimba mukaleta na chisanzo cha zipaso kuziko." Manje ntawi inali ya vipaso voyamba va mpesa. ²¹ Mwaicho bamuna bana yenda naku ona malo kuchokela ku chipululu cha zini kufikila ku Rehobi, pafupi na Lebo Hamathi. ²² Bana yenda kuchokela ku Negevi nakufika ku ku Hebroni. Ahiman, Sheshai, na Talmai, bamubadwe wa Anaki, banali kuja. Manje Hebroni inamangiwa zaka seveni pamene Zoani ikalibe kumangiwa ku Iguputo. ²³ Pamene banafika mu chikwa cha Esikoli, bana juba ntambi ya mutengo wa mpesa. Bana utenga pa nkoli pakati pa gulu yao. Banatenga futi mikuyu. ²⁴ Malo yaja banali kuya itana kuit chikwa cha Esikoli, chifukwa cha mitengo ya mpesa yamene bantu ba israeli bana juba kuja. ²⁵ Pamene panapita masiku fote, bana bwelela kuchokela muku ona malo. ²⁶ Bana bwelela kuli Mose, Aroni, na gulu yonse yabantu ba israeli muchipululu cha Paran, ku Kadeshi. Bana leta mau kuli beve naku gulu yonse, naku ba onesa vishango vochokele kumalo ²⁷ Bana uza Mose, " tinafika ku malo yamene unati tumako. Zoona niyozula na mukaka na uchi. Ivi ndiye vishango vochokele kuja. ²⁸ Manje, bantu bamene bankala kuja niba mpavu. Muzinda ni olimba vipupa ndipo ni ukulu. Tapezako na mutundu wa Anaki kwamene kuja. ²⁹ Bantu ba Amaleki bankala ku Negeve. Ba Heteti, ba Jebuti, na ba Amori bali na manyumba yao kumbali yamalupili muziko. Baku Kenani bankala kumbali kwa manzi namumbali mwa mumana wa Yodani." ³⁰ Mwaicho Kalebua anabauza kuleka kukamba bamene banali pasogolo pa Mose nakukamba, " Tiyeni tikatenge chuma cha malo, chifukwa tikwanisa kuya gonjesa." ³¹ Koma bamuna benangu bamene banayenda naye pamozi banakamba, " sitingakwanise kubamenya aba bantu chifukwa niba mpavu kuchila ife." ³² Mwaicho bana mwaza utenga oyefya bantu ba israeli kamba malo yamene banayenda kuona. Bana kamba, " Malo yamene tina ona ni malo yamene yakudya bantu bamene ba nkalamo. Bantu bonse bamene tina ona kuja ni bantu batali. ³³ Kuja tina ona njomba, mubadwe wa Anaki, bantu bamene banachoka ku njomba. Muku ona kwatu tinali kuoneka monga ntente mukupalanisana nabo, ndiye mwamene tinali kuonekela mu menso mwao, ife."

Chapter 14

¹ Usiku uyo gulu ya musonkano onse inalila mopunda. ² Bantu bonse ba israeli bana pasa mulandu kuli Mose na Aroni. Gulu ya musonkano onse inakamba kuli beve, " asembe chabe tinafa mu malo ya Iguputo, olo muno muchipululu! ³ Nanga nichani Yehova anatibwelesa kuno kumalo kuti tife na lupanga? bakazi batu na bana batu bazavutikilamo. Nichabwino kuli ife kuit tibwelele ku Igupuro?" ⁴ Banali kukambisana wina na muzake, " tiyeni tisanke musogoleli wina, tibwelele naku Iguputo." ⁵ Mwaicho Mose na Aron bana gwesa nkope zao pasogolo pa musonkano wa bantu ba Israeli. ⁶ Yoshua mwana mwamuna wa Nani na Kaleb mwana mwamuna wa Jefunne, bamene banali pali baja banatumiwa kuka ona malo, bana'gamba vovala vao. ⁷ Banakamba ku gulu yonse ya bantu ba israeli. Banakamba, " Malo yamene tinapitamo na ku ona niyabwino maningi. ⁸ Ngati Yehova akomdwela na ife, mwaicho azatipeleka kumalo aya naku tipasa. Malo ya mukaka na uchi. ⁹ Koma musashushane na Yehova, ndipo musayope bantu baku malo yaja, chifukwa bali monga mukate kuli ife. Chitetezo chao chizachosewapo kuli beve, chifukwa Yehova ali na ife. Musaba yop." ¹⁰ Mwaicho mupingo onse unakamba kuti batemeni myala. Koma ulemelelo wa Yehova una onekela pa hema yokumanilanamo kuli bonse bantu ba israeli. ¹¹ Yehova anakamba kuli Mose, " Nikangati pamene aba bantu bazani nyoza? nikangati pamene aba bantu bazakangiwa kuni kulupilila ine, angankale vonse vo onelako mpanvu zanga zamene ninachita pali beve? ¹² Nizaleta chilango pali beve, kubachosa kukupyanika, nakupanga kuchoka ku mutundu wanu ziko yamene izankala ikulu na mpanvu kuchila mwamene balili," ¹³ Mose anakamba kuli Yehova, " Ngati wachita ichi, baku Iguputo bazanvela pali ichi, chifukwa una pulumusa aba bantu kuchoka kuli beve na mpanvu. ¹⁴ Mwaicho naku uza ichi kuli bantu bo nkala mu malo aya. Banvela kuti iwe, Yehova, ulina aba bantu, chifukwa umaoneka menso mpenya. Kumbi yako imaimilila pamwamba pa aba bantu. Uma yenda pasogolo pao mu kumbi muzuba na mu mulilo usiku. ¹⁵ Manje ngati wabapaya aba bantu monga muntu umozi, mwaicho maziko yamene yanavela pali mbili yako yazakamba naku kamba, ¹⁶ Chifukwa Yehova sanapeleke aba bantu ku malo yamene analumbila kuba pasa, aba paya mu chipululu. ¹⁷ Manje, nikupempa, sebenzesa mpanvu zako. Chifukwa unakamba, ¹⁸ Yehova samakwiya musanga ni ozula na chikondi. Amakululukila machimo na volakwa. Sangachosepo machimo ngati aleta chilango cha machimo yamakolo pa mubadwe wao, kuli bachitatu na ba nambala folo mu mubadwe." ¹⁹ Kululuka, nikupempa, chimo ya aba bantu chifukwa cha ukulu wa chipangano chako chokulupilika, monga mwamene umakululukila aba bantu ntau zonse kuchokela pa ntau banali mu Iguputo mapaka na lelo." ²⁰ Yehova anakamba, " Nabakululukila kulingana naku pempa kwako, ²¹ koma zoona, nikali na moyo, na pamene chalo chonse chiza zula na ulemelelo wanga, ²² bantu bonse bana ona ulemelelo wanga na vo onelako mpanvu vamene nina chita mu Iguputo na muchipululu- bapitiliza kuniyesa ine aba ntau zili teni na kusanvelela liu yanga. ²³ Mwaicho nikamba kuti sibaza ona malo yamene ninalumbila ku makolo yao. Kulibe olo umozi wamene ananinyoza aza ya ona, ²⁴ koma chabe wanchito wanga Kaleb, chifukwa ali na muzimu winangu ndipo anikonka na mutima wake onse. Nizamuleta mu malo yamene anayendamo, naba mubadwe wake baza yatenga. ²⁵ (Manje ba Amaleki na baku Kenani banali kunkala mu chikwa.) Mailo pindamukani naku yyenda ku chipululu mu njila yaku mumana wa Reedi." ²⁶ Yehova anakamba na Mose na Aroni. Anakamba, ²⁷ " Nikangati pamene niza lekelela choipa cha gulu yamene inipasa milandu? nanvela kudandaula kwa bantu ba Israeli koshushana na ine. ²⁸ Kamba kuli beve, ' Nikali na moyo, 'akamba Yehova, ' Monga muna kambila mukunvela kwanga, nizachita ichi kuli imwe: ²⁹ Matupi yanu yakufa yazagwa muchipululu, bonse imwe munadamdaula moshushana na ine, imwe bamene muna belengewa mukabelengedwe, nambala yonse ya bantu kuyambila zaka twente zobadwa naku yenda pamwamba. ³⁰ Simiza yenda mumalo yamene nina lonjeza kunkala nyumba yanu, koma chabe Kaleb mwana mwamuna wa Jefunne na Yoshua mwana mwamuna wa Nani. ³¹ Koma bana banu bamene mukamba kuti ndiye bazavutikilamo, nizabapeleka mu malo. Bazapyolamo mu malo yamene mwakana! ³² monga kwaimwe, matupi yanu yakufa yazagwa mu chipululu. ³³ Bana banu bazankala ba busa mu chipululu zaka fote. Bazavalilamo mulandu chifukwa cha vochita va mukangano wanu mpaka kusilila kwa mafupa yanu muchipululu. ³⁴ Monga nambala ya masiku pamene muna yenda kuona malo- masiku fote, mufunika kunyamula chilango cha machimo yanu zaka fote-chaka chimozi cha siku iliyonse, mufunika kuziba mwamene chilili kuli ine kukangana na imwe. ³⁵ Ine, Yehova, nakamba. Vazoona nizachita ichi kuli yonse gulu yo ipa yamene yasonkana pamozi mokangana na ine. Bazachosewapo ndipo kuna baza mwalila." ³⁶ Mwaicho bamu na bamene mose anatuma kuyenda kuona malo, bamene banabwela nakupanga gulu yonse kukangana na Mose naku mwaza mbili yoipa kamba ka malo- ³⁷ aba bamuna bana leta mbili yoipa kamba ka malo bana ponyewa pansi, nakufa na chilango pamenso pa Yehova. ³⁸ Pali abo bamuna banayenda kuona malo, Yoshua chabe mwana mwamuna wa Nani na Kaleb mwana mwamuna wa Jefunne ndiye banasala ba moyo. ³⁹ Pamene Mose anapeleka iyi mbili kuli bantu bonse ba Israeli, banalila maningi. ⁴⁰ Bananyamuka kuseniseni nakuyenda pa

mwamba pa pili nakukamba, " onani, tilipanao, ndipo tizayenda ku malo yamene Yehova anatilonjeza, chifukwa tachimwa." ⁴¹ Koma Mose anakamba, " Nanga nichani muononga lamulo ya Yehova? Simuzakwanisa. ⁴² Osayenda, chifukwa Yehova sali na imwe kuti musagonjesewe na badani banu. ⁴³ Ba Amaleki na baku Kennani baliko kuja, ndipo muzafa na lupanga chifukwa munaleka kukonka Yehova. Mwaicho sazankala na imwe." ⁴⁴ Koma banalimbikila kuyenda ku ziko yakumapili; koma, osati Mose olo bokosi yachipangano cha Yehova vinachoka mu gulu ya musonkano. ⁴⁵ Mwaicho ba Amaleki banabwela, nakuikilapo baku Kenanni banali kunkala kumapili. Bana menya ba Israeli nakuba gonjesa bonse mpaka kufikila ku Homma.

Chapter 15

¹ Mwaicho Yehova anakamba na Mose. Anakamba, ² " Kamba ku bantua ba israeli nakubauza, ' pamene muzayenda kumalo yamene muzayamba kunkala, yamene Yehova azakupasani imwe, ³ mufunika kukonzekala nsembe olo chopeleka cho shoka kuli Yehova, kapena nsembe yo shoka olo nsembe yapa mapwando yanu, yochosa kafungo kabwino kuli Yehova kuchokela pa gulu ya vibeto vanu. ⁴ Mufunika kupasa kuli Yehova nsembe yoshoka pamozi na nsembe ya mbeu ya chakumi cho gaya cha fulaulo yo sankaniza na cha nambala folo cha mafuta yo tikama. ⁵ Mufunika futi kupasa na nsembe yoshoka, olo chopeleka, cha nambala folo cha mafuta yo tikama ya vinyu cha nsembe ya chakumwa kuli mbelele iliyonse. ⁶ Ngati mupasa nsembe ya nkosa, mufunika kukonzekala nsembe ya mbeu ya chibili-pachakumi pa chogaya ya fulaulo yosankaniza na chachitatu cha mafuta yotikama. ⁷ Ya nsembe ya chakumwa, mufunika kupasa chachitatu cha mafuta yotikama ya vinyu. Izachosa kafungo konunkila kuli Yehova. ⁸ Ngati mwakonzabulu munga nsembe yoshoka olo chopeleka chokwanilisa kulumbila, olo munga nsembe ya chiyanjano kuli Yehova, ⁹ mwaicho mufunika kupasa pamozi na bulu nsembe ya mbeu na mafuta yotikama yan'gono. ¹⁰ Mufunika kupasa munga nsembe ya chakumwa vinyu vin'gono, munga nsembe yoshoka pa mulilo, kuchosa kafungo kabwino kuli Yehova. ¹¹ Ifunika kuipanga munjila iyi bulu iliyonse, ku mbelele iliyonse, nakuli mbelele imuna iliyonse olo mbuzi zing'ono. ¹² Chopeleka chili chonse chamene mukonzabulu na kupasa ifunika kupanga munga nakambila apa. ¹³ Bonse bobadwila kuno afunika kuchita ivi vintu munga mwamene umu, ngati aliyense aleta nsembe yoshoka mu mulilo, kuchosa kafungo kabwino kuli Yehova. ¹⁴ Ngati mulendo ankala naimwe, olo aliyense wamene azankala naimwe mu mubadwe onse wa bantu banu, afunika kupanga nsembe yoshoka pa mulilo, yochosa kafungo kabwino kuli Yehova. Afunika kuchita munga mwamene muchitila. ¹⁵ Kufunika kunkala lamulo yopalana pa gulu na ku mulendo wamene ankala naimwe, lamulo yonkalilila mu mubadwe onse wa bantu banu. Munga mwamene mulili, ndiye mwamene otandala afunika kunkalila naimwe. Afunika kuchita munga mwamene muchitila pamenso pa Yehova. ¹⁶ Lamulo imozi mozi ifunika kusebenza kuli imwe na kuli mulendo wamene ankala naimwe." ¹⁷ Nafuti Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ¹⁸ " Kamba ku bantu ba israeli naku bauza, ' ngati mwabwela ku malo kwamene nizakupelekani, ¹⁹ ngati mwadya vakudya vochokelela mumalo, mufunika kupasa nsembe nakuibwelesa kuli ine. ²⁰ Kuchokela ku flaulo yofufumuka yoyambilila yanu, mufunika kupasa mukate ku unyamula mumwamba munga nsembe yonyamula yochokela mukugaya pansi. Mufunika kuinyamula munjila iyi. ²¹ Mufunika kunipasa nsembe yonyamula mumubadwe wabantu banu bonse kuchokela ku fulaulo yofufumuka yo yamba. ²² Muzayamba kuchimwa ntau zina mosaganizila kuchita mwamene mwachitila, ngati simunanvelele yonse aya malamulo yamene nakamba kuli Mose- ²³ vonse vamene ninakulamulilani kupitila muli Mose kuchokela pasiku yamene niyamba kukupasani malamulo nakuyenda musogolo kupita mumubadwe wanu. ²⁴ Munkani yochimwa mosaziba na gulu sina zibe, mwaicho gulu yonse ifunika kupasa mwana wa bulu umozi munga nsembe yoshoka yochosa kafungo kabwino kuli Yehova. Pamozi na ivi mufunika kupanga nsembe ya mbeu na nsembe yachakumwa, munga mwa lamulo, na mbuzi imuna imozi munga nsembe ya chimo. ²⁵ Wansembe afunika kuyelesela gulu yonse ya bantu ba israeli. Baza kululukiwa chifukwa chimo inali chabe kusokoneza. Baleta chopeleka chao, nsembe yoshoka pa mulilo kuli ine. Babwelesa nsembe yao ya chimo kuli ine kamba kaku sokoneza kwao. ²⁶ Mwaicho gulu yonse yabantu ba israeli izakululukiwa, na balendo bamene ba nkala nabo, chifukwa bantu bonse banachita chimo mosaziba. ²⁷ Ngati muntu achimwa mosaziba, mwaicho afunika kupasa mbuzi ikazi ya chaka chimozi munga nsembe ya chimo. ²⁸ Wa nsembe afunika ku yelesela pamenso pa Yehova chifukwa cha muntu wamene achimwa mosaziba. Uyo muntu azakululukiwa ngati kuyelesela kwachitka. ²⁹ Mufunika kunkala na lamulo imozi mozi nakuli muntu achita chintu chili chonse mosaziba, lamulo imozi mozi kuli obadwila pakati pa bantu ba israeli na kuba lendo bamene bankala nabo. ³⁰ Koma muntu wamene achita chili chonse cholakwika, olo niobadwila kumalo kwanu olo ni mulendo, aninyoza ine. Uyo muntu afunika kuchosewa kubantu bake. ³¹ Chifukwa anyoza mau yanga nakupwanya malamulo yanga, uyu muntu afunika kuchosewelatu. Chimo yake izankala pali eve." ³² Pamene bana ba israeli banali mu chipululu, bana peza mwamuna adoba nkuni pa siku ya sabata. ³³ Baja bana mupeza banamuleta kuli Mose, Aroni, na gulu yonse. ³⁴ Bana musunga mokomela chifukwa benze bakalibe kukamba vamene bafunika kumuchita. ³⁵ Mwaicho Yehova anakamba kuli Mose, " uyo mwamuna afunika ku paiwa. Gulu yonse ifunika kumutema myala panja pa musonkano." ³⁶ Mwaicho gulu yonse inamuleta panja pa musonkano nakumutema myala mpaka afa munga mwamene Yehova analamulila Mose. ³⁷ Nafuti Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ³⁸ " Kamba kuba mubadwe wa israeli naku ba lamula kuti bapange kanyula ko kobeka kumbali kwa mikanjo yao, kukobeka kumbali iliyonse nacho onelako cho buluwa. Bafunika kuchita ichi mu mubadwe wa bantu bao bonse. ³⁹ Chizankala chokumbukisilako kuli imwe, pamene muyanganako, yonse malamulo yanga, kuyanyamula kuti

musayangane pamutima wanu na mumenso mwanu nakuchita uhule kwaimwe mweka kuli beve. ⁴⁰ Chita ichi kuti munga kumbukile nakunvelela malamulo yanga yonse, mwaicho kuti mungankale holy, kusungiwa kuli ine, mulungu wanu. ⁴¹ Ndine Yehova mulungu, anakuchosani mumalo ya Iguputo, kunkala mulungu wanu. Ndine Yehova mulungu wanu."

Chapter 16

¹ Kora mwana mwamuna wa Izhar mwana mwamuna wa Kohati mwana mwamuna wa Levi, pamozi na Datani na Abiramu mwana mwamuna wa Eliab, na Oni mwana mwamuna wa Peleti, wa mubadwe wa Reubeni, anaika pamozi bamuna. ² Bana yamba kukangana na Mose, pamozi na bamuna bena kuchokela pa bantu ba israeli, 250 basogoleli ba pa gulu banali bozi-bika mamembala bamu gulu. ³ Banazi unjika pamozi naku konka Mose na Aroni. Bnakamba kuli beve, " mwaenda patali maningi! gulu yonse yagabanika, aliyense pali beve, na Yehova ali nabo. Nanga nichani muzi ika pamwamba mweka kuchila gulu ya Yehova yonse?" ⁴ Pamene Mose ananvela ivi, anagwesa nkope yake pansi. ⁵ Anakamba na Kora pamozi nabamene anali nabo, " Kuseni Yehova azatizibisa bamene bali bake na boyela kuli eve. Azaleta uyo muntu pafupi na eve. Wamene asanka azamuleta pafupi kuli eve mwine eka. ⁶ Chita ichi, Kora na gulu yako. Panda chibelengelo ⁷ mailo naku ika mulilo na mafuta yonunkila kuli beve pamenso pa Yehova. Wamene Yehova asanka, uyo muntu azankala oyela kuli Yehova. Mwayenda patali maningi, imwe ba mubadwe wa Levi." ⁸ Nafuti Mose anakamba kuli Kora, " manje nvelani, imwe ba mubadwe wa Levi: ⁹ nichitnu chin'gono kuti mulungu wa israeli akupatulanikuchoka pa guluya israeli, naku kuletani pafupi kuli eve eka, kuchita nchito mu kachisi ya Yehova, naku imilila pasogolo a gulu naku musebenzela? ¹⁰ Akuletani pafupi, nabonse bamene mubadwa nabo, ba mubadwe wa Levi, muli nabo, ndipo mufuna udindo wa unsembe! ¹¹ Mwaicho iwe na bonse muli nabo mwa unjikana mushushana na Yehova. Nanga Aroni ni ndani wamene muvutana naye?" ¹² Mwaicho Mose anaitana Datani na Abiramu, bana bamuna ba Eliabu, koma banakamba, " sitizabwela. ¹³ Nanga nichintu ching'ono kuti unati chosa mu malo ya mukaka na uchi, kuti paya muchipululu? Mwaicho ufuna kuzipanga olamulila pali ife! ¹⁴ kuikilapo, si unatilete mu malo ya mukaka na uchi, olo kuti pasa minda na minda za mpesa monga vopyanika watu. Manje ufuna kuti nama namalonjezo ya boza? sitizabwela kuli iwe." ¹⁵ Mose anakalipa naku kamba kuli Yehova, " Musalemekeza nsembe yao. Sininatenge bulu umozi kuli beve, ndipo sinina pange ngozi kuli aliyense kuli beve." ¹⁶ Mwaicho Mose anakamba kuli Kora, " Mailo iwe na gulu yako muyende pamenso pa Yehova-iwe na beve, na Aroni. ¹⁷ Aliyense pali imwe atenge choikilapo na mafuta yonunkila poikila. Mwaicho mwamuna aliyense aleta kuli Yehova choikilapo mafuta yonunkila, 250 poikila. Imwe na Aroni, futi, aliyense afunika kuleta choikilapo chake." ¹⁸ Mwaicho mwamuna aliyenseanatenga choikilapo chake, nakuikapo mulilo, nakuikamo mafuta yonunkila, naku imilila pa komo yaku hema yokumanilanamo pamozi na Mose na Aroni. ¹⁹ Kora ana unjika gulu yokangana na Mose na Aroni pa komo ya hema yokumanilanamo, na ulemelelo wa Yehova unaonekela ku gulu yonse. ²⁰ Mwaicho Yehova anakamba na Mose na Aroni: ²¹ " Zipatuleni kuli iyi gulu kuti niba ononge pamene apa." ²² Mose na Aroni banagwesa nkope zao nakukamba, " Mulungu, Mulungu wa muzimu ya bantu, ngati muntu umozi achimwa, nanga ufunika kukalipa na gulu yonse?" ²³ Yehova anayanka kuli Mose. Anakamba, ²⁴ " Kamba ku gulu. Kamba, ' chokani mu mahemaya Kora, Datani, na Abiramu." ²⁵ Mwaicho Mose anayenda kuli Dtani na Abiramu; bakulu bakulu ba Israeli banamukonka. ²⁶ Anakamba ku gulu nakubauza, " manje chokani mu mahema ya aba bantu bo ipa musatenge chili chonse chitu chao, kuti musa onongekele pamozi mumachimo yao." ²⁷ Mwaicho gulu kumbali zonse za ma hema ya Kora, Datani, na Abiramu bana basiya. Datani na Abiramu bana choka panja naku imilila pa makomo ya ma hema yao, na bakazi bao, bana bao bamuna, na bang'ono bao. ²⁸ Mwaicho Mose anakamba, " Mwaichi muzaziba kuiti Yehova ananituma kuchita nchito izi zonse, chfukwa sininazichite mukufuna kwanga. ²⁹ Ngati aba bamuna bafa imfa yozifela monga mwamene imankalila, ninshi Yehova sananitume. ³⁰ Koma ngati Yehova apanga chintu china chanyowani, na chalo chiseguke nakubamela, na vonse vintu bali navo, nakuyenda bali na moyo mu mugodi, mwaicho mufunika kuziba kuti aba bamuna banyoza Yehova." ³¹ Pamene Mose anasiliza kukamba mau yonse, pansi panaseguka pamene banali baja bamuna. ³² Chalo chinasegula kamwa kake nakuba mela, mabanja yao, na bonse bantu banali ku mbali ya Kora, pamozi nama katundu yao. ³³ Mwaicho beve na makatundu bana gwela mu mugodi ba moyo. Chalo chinaba vininkila, naku onongeka kuchoka pa gulu. ³⁴ Israeli yonse banali kubazunguluka banataba kuchoka ku kulila kwao. Bana punda, " chalo chingatimele naife!" ³⁵ Mwaicho mulilo unayaka kuchoka kuli Yehova nakuononga bamuna 250 bana pasa mafuta yonunkila. ³⁶ Futi Yehova anakamba na Mose nakukamba, ³⁷ " Kamba kuli Eleazar mwana mwamuna wa Aroni wansembe kuti atenge vosungilamo kuchoka muchimbilimbili, chifukwa vosungilamo nivoyela kuli ine. Mu uze kuti amwaze malasha patali patali. ³⁸ Tenga vosungilamo va abo bamwalilachifukwa cha chimo. Vipangiwe mbale zokokomela mongs zovininkila pa guwa. Baja bamuna banazipasa kuli ine, mwaicho nizoyela kuli ine. Zizankala chozibilako kuli kupezekao kwanga kuli bantu ba israeli." ³⁹ Eleazar wansembe anatenga vosungilamo va bulonze vame ne bana sebenzesa bamuna bamene banashokewa, nakuvikokomela kupanga vovininkila pa guwa, ⁴⁰ kunkala chikumbuso ku bantu ba Israeli, kuti kusa nkale mulendo aliyense wamene sali wa mubadwe wa Aroni azabwela kushoka mafuta yonunkila kuli pamenso pa Yehova, kuti basankale monga Kora na gulu yake- monga mwamene

Yehova analamulila kupitila muli Mose. ⁴¹ Koma kuseni kuna konkapom gulu yonse ya bantu ba Israeli inadandaula kuli Mose na Aroni. Bana kamba, " Mwapaya bantu ba Yehova." Mwaicho ⁴² vinachitika pamene gulu ina unjikana mokangana na Mose na Aroni, banali kuyangana ku hema yokumanilanamo na, kuona, kumbi inavininkila. Ulemelelo wa Yehova unaonekela, ⁴³ na Mose na Aroni bana bwela pa sogolo pa hema yokumanilanamo. ⁴⁴ Mwaicho Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ⁴⁵ " chokani pasogolo pa gulu iyi kuti ninga baononge pamene apa." Mwaicho Mose na Aroni banagwesa nfeshi zao pansi. ⁴⁶ Mose anakamba kuli Aroni, " Tenga choikilamo, ikapo mulilo kuchoka pa guwa, ikapo mafuta yonunkila, nyamula musanga musanga upeleke ku gulu, na kupanga choyelesela kuli beve, chifukwa kukalipa kuchokela kuli Yehova. Chigumula chayamba." ⁴⁷ Mwaicho Aroni anachita monga mwamene Mose anakambila. Anatamangila pakati pa gulu. Chiumula chinayamba kudala kumwazikana pa bantu ba Israeli, mwaicho anaikapo mafuta yonunkila nakuyelesela bantu ba Israeli. ⁴⁸ Aroni anaimilila pakati ka bakufa na bamoyo; mwaichi chigumula chinaleka. ⁴⁹ Abo banafa na chigumula banali 14,700 mu nambala, kuchoselako banafa mu nkani ya Kora. ⁵⁰ Aroni anabwelela kuli Mose pa komo yaku hema yokumanilanamo, nachigumula chinasila.

Chapter 17

¹ Yehova anakamba kuli Mose. Anakamba, ² " kamba kubantu ba israeli nakutenga nkoli kuchokela kuli beve, imozi kuli mubadwe wa mutundu uli onse, nkoli zili tweluvu. Lembani zina ya mwamuna uli onse pa nkoli yake. ³ Ufunika kulemba zina ya Aroni pa nkoli ya Levi. Kufunika kunkala nkoli imozi ku musogoleli aliyense kuchokela ku mubadwe wa mutundu wake. ⁴ Mufunika kuika nkoli mu hema yokumanilamo pa sogolo pa malamulo yachipangano, kwamene nimakumana naiwe. ⁵ Kuzachitika kuti nkoli ya mwamuna wamene niza sanku izamela ntambi. Niza lengesa madandaulo ya bantu ba isreali kuleka, yamene bakamba kuli iwe." ⁶ Mwaicho Mose anakamba ku bantu ba Israeli. Bonse basogoleli bana mupasa nkoli zao, nkoli imozi ya musogoleli aliyense, yosankiwa kuchokela mu mutundu wa makolo, nkoli zili tweluvu zonse pamozi. Nkoli ya Aroni nayeve inalipo. ⁷ Mwaicho Mose anaika nkoli pamenso pa Yehova mu hema ya malamulo yachipangano. ⁸ Siku yokonkapo Mose anayenda mu hema ya malamulo yachipangano, onani, nkoli ya Aroni inamela ntambi. Inakulu ntambi nakuchosa nakuchosa matepo na maluba yanali pafupi nakuseguka! ⁹ Mose analeta nkoli zonse kuchosa pamenso pa Yehova kuli bantu bonse ba Israeli, na mwamuna aliyense anatenga nkoli yake. ¹⁰ Yehova anakamba kuli Mose, " Ika nkoli ya Aroni pasogolo pa malamulo yachipangano. Isunge monga cho onelako chakulakwa kwa bantu ba Israeli bamene bana panga mukangano kuti munga silize madandaulo kuli ine, olo baza mwalila." ¹¹ Mose anachita monga mwamene Yehova anamulamulila. ¹² Bantu Israeli banakamba kuli Mose na kunena, " Tizafa kuno. Tiza onongeka tonse! ¹³ Aliyense wamene azabwela, naku yenda kuli tempele ya Yehova, azafa. Nanga tifunika tonse kufa?"

Chapter 18

¹ Yehova anakamba, kuli Aroni, " iwe, bana bako bamuna, na makolo ba mutundu wako muzankala bo yanganila machimo yonse yopangiwa mokangana na malo yoyela. Koma chabe iwe na bana bako bamuna bamene uli nabo muza nkala bo yanganila machimo yonse yapangiwa na aliyense pa ba nsembe. ² Monga kuma membala ba mutundu wa Levi, makolo ya mu tundu wako, ufunika kubwela nabo kuti bankale na iwe na kuku tandiza pamene iwe na bana bako bamuna musebenza pa sogolo pa hema ya malamulo yachipangano. ³ Bafinika ku kusebenzela na na hema yonse. Mwaicho, sibafunika kubwela pafupi na chili chonse mu malo yoyela olo chogwililila ku guwa, chifukwa iwe na beve mungafe. ⁴ Bafunika kunkala pamozi naiwe nakusunga hema yokumanilamo, kunchito zonse zamu hema. Mulendo safunika kubwela pafupi naiwe. ⁵ Ufunika kusamalila malo yoyela na yaku guwa kuti kukalipa kwanga kusabwele pa bantu ba Israeli nafuti. ⁶ Ona, ine mwine nasanka mamembala banzako balevi kuchokela pa mubadwe wa Israeli. Bali monga mpaso kuli iwe, bopasiwa kuli ine kuchita nchito zaku hema yokumanilanamo. ⁷ Koma iwe chabe na bana bako bamuna ndiye munga chite nchito zau nsembe zaku guwa na vonse vili mukati mwa nyula. Imwe mweka mufunika kukwanilisa izo nchito. Nikupasani unsembe monga mpaso. Mulendo aliyense wamene afendela pafupi afunika kupaiwa." ⁸ Mwaicho Yehova anakamba kuli Aroni, " Ona, nakupasa nchito yo yanganila nsembe zobwela kuli ine, na nsembe zonse zoyela zamene bantu Israeli bapasa kuli ine. Napasa izi nsembe kuli iwe na bana bako bamuna monga mbali yanu ya ntau zonse. ⁹ Izi ziza nkala zaku kuchokela ku vintu vo yela vosungiwa kuchoka kumulilo. Kuchokela ku nsembe iliyonse yao-nsembe iliyonse ya mbeu, nsembe iliyonse ya chimo, na nsembe iliyonse yakulakwa-nizoyelesewa kuli iwe na bana bako bamuna. ¹⁰ Izi nsembe nizoyela maningi; mwamuna aliyense afunika kuidya, chifukwa nizo yela kuli imwe. ¹¹ Izi ni nsembe zamene ziza nkala zanu, patulaniponi kuchoka pa mpaso zao za nsembe yo weyula za bantu ba Isrseli. Nazipasa kuli iwe, bana bako bamuna, na bana bako bakazi, monga mbali yanu ya ntau zonse. Aliyense ali oyela monga mwa mwambo mu banja yanu angadyeko izi nsembe. ¹² Yonse mafuta yabwino, vonse vinyu vabwino va nyowani na mbeu, vipaso voyamba vamene bantu ba pasa kuli ine-vonse vintu vamene ninakupsani. ¹³ Voyambilila kupya vochoka mumalo yao, vamene baleta kuli ine, vizankala vako. Aliyense mubanja yako wamene ali oyela angadyeko ivi vintu. ¹⁴ Chilichonse chintu chopeleka mu Israeli chizankala chako. ¹⁵ Chilichonse chamene chisegula mimba, vobadwa voyamba vonse vamene bantu bapasa kuli Yehova, pamozi bantu na vinyama, vizankala vako. Koma, bantu bafinika kuombola mwana mwamuna obadwa oyamba, ndipo bafunika kuombola vobadwa voyamba vimuna pa vinyama vosayela. ¹⁶ Ivo vamene baza gula bantu vifunika kuguliwa futi ngati vakwanisa mwenzi umozi. Mwaicho bantu bangavigule futi, pamutengo wama shekele yali faivi, yolingana na ma gelashe yali twente. ¹⁷ Koma chobadwa choyamba cha ngombe, olo chobadwa choyamba cha mbelele, olo chobadwa choyamba cha mbuzi-simufunika kuombola ivi vinyama; nivopatulika kuli ine. Mufunika kuwaza magari yao pa guwa naku shoka mafuta yake monga nsembe yoshoka, kafungo kabwino kuli Yehova. ¹⁸ Nyama yao izankala yanu. Monga nganga yoweyula nachibelo chaku kwanja ya manja, nyama yao izankala yanu. ¹⁹ Zonse nsembe zoyela zamene bantu ba Israeli bapasa kuli Yehova, nakupasa iwe, na bana bako bamuna naku bana bako bakazi bamene bali na iwe, monga mpaso yo yendelela. Nichipangano chamuyayaya cha sauti, chipanagano chaika pamozi chamuyayaya, pamenso pa Yehova pamozi kuli imwe na bamubadwe bako bamene uli nabo." ²⁰ Yehova anakamba kuli Aroni, " Simuzankala na chopyanika mu malo ya bantu. Ndine mbali yanu na chopyanika chapa bantu ba Israeli. ²¹ Kubamubadwe wa Levi, ona, napasa chakumi chonse chamu Israeli kunkala chopyanika chao mukubwezela nchito zamane bachita mukusebenza ku hema yokumanilamo. ²² Kuyambila manje bantu ba Israeli sibafunika kubwela pafupi na hema yokumanilanamo, olo bazankala na chimo nakufa. ²³ Ba Levi bafunika kuchita nchito yaku hema yokumanilanamo. Bazankala boyanganila machimo yali yonse ya uko. Iyi izankala lamulo yonkalilila mu mubadwe wa bantu banu. Pa bantu ba Israeli sibafunika kunkala na chopyanika. ²⁴ Ku chakumi cha bantu ba Israeli, chamene ba peleka monga mpaso kuli ine -ni ivi vamene napasa kuli ba Levi monga chopyanika chao. Ndiye chifukwa chamene ninakambila kuli beve. ' sibafunika kunkala na chopyanika pa bantu ba Israeli.'" ²⁵ Yehova anakamba kuli Mose nakukamba, ²⁶ " ufunika kukamba naba Levi naku kamba kuli beve, ' Ngati wapokelela kuchokela kubantu ba Israeli chakumi chamene napasa kuli iwe kuchokela kuli beve kunkala chopyanika chako, uzapasa chosonka kuchokela kuli cheve kuli Yehova, chakumi cha chakumi. ²⁷ Chopeleka chako chifunika kuoneka monga chinali chakumi cha mbeu kuchokela ku vukutwa pansu olo chopangiwa kuchokela pavofyanta pa vinyu. ²⁸ Mwaicho naiwe ufunika kupasa chosonka kuli Yehova kuchokela ku chakumi chonse chamene upokelela kuchokela ku bantu ba Israeli. Kuchokela kuli beve ufunika kupasa chopeleka chake kuli Aroni wansembe. ²⁹ Kuchokela pa mpaso zonse zamene upokelela, ufunika kusunika kuli Yehova. Ufunika kuchita ichi kuchokela ku vonse vabwino na vintu voyela maningi vamene vapasiwa kuli iwe.' ³⁰ Mwaicho

ufunika kukamba kuli beve, ' ngati wapasa yabwino pali yeve, mwaicho ifunika kubelengewa kuli ba Levi monga chopanga cho chokela pa vokutwa pansi na vofyanta ku vinyu. ³¹ Ungadye vosalapo pa mpaso mumalo yali yonse,iwe na banja yako, chifukwa nimalipilo yanu ku nchito yanu yanu hema yokumanilanamo. ³² Simuzankala na kulakwa kuli konse mukadya nakumwa, ngati mwapasa kuli Yehova vabwino pali vamene mwalandila. Koma simufunika kuona monga ni nsembe zoyela ya bantu ba Israeli, olo mungafe."

Chapter 19

¹ Yehova anakamba kwa Mose ndi Aroni. Anakamba, Iyi ndiye lamulo, lamulo yamene nnipeleka kwa imwe: ² Kambani ku banthu ba Israele kuti bafunika kubwelesha ng'ombe yikazi yo sweta yamene ilibe ulema, ndiponso yamene siinatengepo joko. ³ Pelekani ng'ombe kwa Eliezara wansembe. Ndipo aibwelese kunja kwa musasa, Ndipo munthu winangu aipaye pasogolo pake. ⁴ Eliezara wansembe afunika kutengako magazi na njala zake na kuwanzia kali seveni kusogolo kwa tenti yokunanilamo. ⁵ Ng'ombe ifunika kuishoka pa menso pake—chikopa chake, munofu, ndi magazi nava mukati, vifunika kushokewa. ⁶ Wansembe afunika kutenga mutengo wa mukunguza, hisope, ndi nsalu yosweta, nakuiponya yonse mukati mwa ng'ombe yoshokewa. ⁷ Ndipo afunika kuchapa vovala vake na kusamba mu manzi. Pamenepo angabwele mu musasa, mwamene azankala osayela kufikila mu mazulo. ⁸ Munthu wamene washoka ng'ombe afunika kuchapa vovala vake mu manzi na kusamba mu manzi. azankala osayela kufikila mu mazulo. ⁹ Muntu wamene ali oyelesedwa afunika kufaka pamozi pulusa ya ng'ombe na kuifaka panja pa musasa mu malo yoyelesedwa. Aya mapulusa yafunika kusungila banthu ba Israele. Bazasankaniza pulusa ndi manzi zoyelesela ku uchimo, chifukwaa pulusa inachokela ku nsembe yauchimo. ¹⁰ Muntu wamene afaka pamozi pulusa ya ng'ombe afunika kuchapa vovala vake. Azankala osayela kufikila mumazulo. Iyi izankala lamulo yamuyayaya kwa bantu ba Israele na bonse balendo bamene bankala nawo. ¹¹ Aliyense azagwila tupi yakufa ya muntu aliyense azankala osayela masiku yali seveni. ¹² Muntu waso afunika kuziyelesa eka pa siku ya chitatu na pasiku ya namba seveni. Ndipo azankala woyela. Koma ngati sazaziyelesa eka pasiku yachitatu, sazankala woyelesedwa pasiku ya seveni. ¹³ Aliyense azagwila munthu wakufa, tupi ya munthu uja wakufa, ndipo sazaziyelesa eka, Uyo munthu aononga chalichi ya Yehova. Uyo munthu afunika kuchosedwa mu Israele chifukwa manzi yoyeleza siyanawazike pali yeve. Azankala wosayelesedwa; kusayelesedwa kwake kuzasala pali yeve. ¹⁴ Iyi ndiye lamulo kwa munthu wamene afela mu tenti. Alionse wamene ayenda mu tenti na alionse ali kudala mutenti azankala wosayela masiku seveni. ¹⁵ kontena iliyonse izankala ilibe chovininkila izankala yosayela, ¹⁶ Molinganiza, muntu alibonse ali panja pa tenti wamene agwila aliyense wamene apaidwa na panga, tupi iliyonse yakufa, fupa ya muntu, kapena manda, uyo munthu azankala osayela masiku yali seveni. ¹⁷ Chitani ichi ku muntu wosayela: Tengani pulusa kuchokela ku nsembe ya kuyelesa na kusankaniza ndi manzi yabwino mu musuko. ¹⁸ Muntu oyelesedwa afunika kutenga hisope, kuingenesa mu manzi, ndi kuwazya pa tenti, pa makontena yonse yali mukati mwa tenti, na pabanthu banali banali mwamene umo, na munthu alionse anagwila mafupa, kapena wamene anapaidwa, wamene anafa, kapena manda. ¹⁹ Pa usiku wautatu na pausiku wa seveni, muntu woyela afunika kuwazya pa munthu wosayela. Pa usiku ya namba seveni muntu wosayela afunika kuziyelesa eka. Afunika kuchapa vovala vake na kusamba mumanzi. Kumazulo azankala woyela. ²⁰ Koma alionse azasala wosayela, wamene akana kuziyelesa eka, Uyo muntu afunika kuchosedwa pa munzi, chifukwa aononga chalichi ya Yehova. Manzi yoyeleza siyanawaike pali eve; azankala wosayela. ²¹ Iyi izankala lamulo yonkazikika kwa ivi vintu. Wamene atilila manzi yo yelesa afunika kuchapa vovala. Wamene agwila manzi yoyeleza azankala osayela kufikila mumazulo. ²² Vili vonse wamene muntu wosayela agwila vizankala wosayela. Muntu azavingwila azankala wosayela kufikila mumazulo."

Chapter 20

¹ Sono banthu ba Israeli, munzi wonse, banayenda mu chipululu cha Zini mu mwezi woyamba; banankala ku Kadesi. Kwamenekuja Mirriamu anamwalila ndipo bana mushika. ² Kunalibe manzi ya bamumunzi, chonco banakumana pamozi mukushushana na Mose ndi Aroni. ³ Banthu banakangana na Mose. Bana kamba, "Chinali bwino ngati naife tinafa pamene ba bale bathu ma Israeli banafa mamenso ya Yehova. ⁴ Nichifukwa chani waleta munzi wa Yehova muno muchipululu kufela kuno, ife na nyama zathu? ⁵ Nichifwa chani unatuchosela mu Ziko ya Igupto kuti bwelesa kuno kumalo koipa? kulibe malo yoshangamo, mukuyu, mpesa kapena makangaza, ndipo kulibe manzi yakumwa." ⁶ Mose na Aroni banachoka nakuyenda kusogolo kwa musonkano. Banayenda pongenela pa tenti yokumanilamo na kugona cholangana pansi. ⁷ Yehova anakamba na Mose na kuti, ⁸ "Tenga ndodo na kusonkanisa banthu, iwe na Aroni mubale wako. Kamba ku chimwala pamenso yabo, ndipo uchiuze chimwala kuti chichose manzi. uzachosa manzi yabo kuchokela mu mwala, ndipo uzapasa ku munzi navo vosunga vabo kuti bamwe. ⁹ Mose anatenga ndondo pamenso pa Yehova, monga mwamene Yehova anamulamulila kuti achite. ¹⁰ Ndipo Mose ndi Aroni bana sonkanisa banthu bonse pamozi pasogolo pa mwala. Mose anakamba kuti, "Nvelani manje, imwe osanvela. Mufuna kuti tikubweleseni manzi kuchokela ku mwala uyu? ¹¹ Ndipo Mose ananyamula kwanja na kumenya pa mwala kabili na ndondo yake, na manzi yambiri yanachoka. Bamumuzi banamwa, na zobeta zabo zinamwa. ¹² Koma Yehova anakamba kwa Mose na Aroni, "Chifukwa imwe simunanikulupilie kapena kunilemekeza Ine monga Oyela pa menso ya bathu ba Aisraeli, simuzababwelesa aba banthu ku malo yamene nabapasa iwo." ¹³ Yano malo banali kuyaitana kuti manzi ya Meriba chifukwa banthu ba ku Israele bana kangana na Yehova, ndipo anazilangiza kuli beve kuti ni woyela. ¹⁴ Mose anatuma wopeka utenga kuchoka ku Kadesi to mfumu yaku Edomu: Mubale wako Israeli akamba kuti, "Uziba vonse vovuta vamene vachitika kwa Ife. ¹⁵ Uziba kuti makolo yathu bana yenda ku Igupto nakunkala mu Igupto ntawi yaitali. Aigupto banativutisa moipa pamozi na makolo banthu. ¹⁶ Pamene tinaitanila kuli Yehova, ananvela mau yathu na kutuma mungelo na kutuchosa mu ziko ya Aigupto. Onani,tili mu Kadesi, Muzi wamene uli mumbali ya malo yanu. ¹⁷ Nipempa kwa Inu kuti mutivomeleze kupitako mumalo mwanu. Sitizapita mu munda kapena munda wa mpesa, ndipo sitizamwa manzi yamu visime vanu, tizapitila munjila ya mfumu. Sitizapatukila ku kwanja kwa manja kapena ku yamanzele panka tikapitilila malile yanu." ¹⁸ Koma mfumu yaku Edomu inayanka kuti, Usapitile pakati pano. chifukwa ukachita ichi, nizabwela na lupanga Kuzakumenya. ¹⁹ Ndipo banthu ba Israyeli banakamba naye, "tizapita mu njila. koma ife na zobeta zanthu tikamwa manzi yanu, tizayalipilila. Tilekeni tiyendemo na mendo, sitizachitamo kanthu kalikonse." ²⁰ Koma mfumu yaku Edomu inayanka, "Simuzapitamo."Ndipo mfumu ya Edomu inabwela kuyamba ndi Israele na kwanja kwa mphamvu na masoja yambili. ²¹ Mfumu yaku Edomu inakana kubavomeleza ba Israeli kupitilila kumalile kwawo. Chifukwa cha ichi, ma Israeli bana patukila kumalo kwa Edomu. ²² Ndipo banthu banayenda ulendo kuchoka ku Kadesi. Bathu ba Israeli, na gulupu yonse, bana bwela ku lupili lwa Hori. ²³ Yehova anakamba kuli Mose na Aroni palupili lwa Hori, ku malile kwa ziko ya Edomu. Anakamba, ²⁴ "Aroni ankale pamozi na bathu bake, chifukwa sazangena mu malo yamene napasa banthu baku Israeli. Ichi nichifukwa simunavelele mau yanga ku manzi ya Meriba. ²⁵ Tenga Aroni na Eleazara mwana wake mwamuna, na kubabwelesa kulupili lwa Hori. ²⁶ Tengan vovala vansembe va Aroni kuli eve nakuvalika Eleazara mwana wake mwamuna. Aroni afunika kufa nakumubwelesa ku bathu bake kwamene uko." ²⁷ Mose anachita mwamene Yehova anamuuzila. Banayenda pamwamba palupili lwa Hori pamenso pa banthu bonse. ²⁸ Mose anavula Aroni vovala vake nakuvalika Eleazara mwana wake mwamuna. Aroni anafa kwamene uko pamwamba pa lupili. Ndipo Mose na Eleazara banabwela pansi. ²⁹ Pamene Muzi bonse unaona kuti Aroni amwalila, Ziko yonse inamulila Aroni masiku yali feti.

Chapter 21

¹ Pamene makanani mfumu ya Aradi, anankala ku Nevevi, ananvela kuti Israele anabwela na njila ku Atarimu, Anamenyana nama Israeli nakutenga benangu kunkala womangidwa. ² Israeli analumbila kuli Yehova na kuti, "Mukatipasa kugonjesa aba banthu, ndipo tizaonengelatu mizinda yawo." ³ Yehova ananvela mau yaba Israele na kubapasa chigonjeso pali Akanani. Ndipo banabaonongelatu na mizinda yawo. Ayo malo banayakamba kuti Horoma. ⁴ Ndipo banayenda kuchoka ku pili ya Hori na njila yaku nyanja ya Reeds nakuzunguluka malo ya Edomu. Ndipo banthu banankala wofoka munjila. ⁵ Banthu banakamba mosushana na Mulungu na Mose: "Nichifukwa chani watichosela mu Igupto kuti tifele mu chipululu? Kulibe buledi, kulibe manzi, ndipo tizonda ivi vakudya voipa." ⁶ Ndipo Yehova anatuma njoka zaululu pakati pa bathu. Njoka zinaluma bathu; bambili banthu banamwalila. ⁷ Banthu banabwela kwa Mose na kukamba, "Twachimwa chifukwa takamba vosushana naye Yehova na Iwe. Pempela kuli Yahova kuti azitenge njoka kuchoka pali ife." Ndipo Mose anabapempelela banthu. ⁸ Yehova anakamba kuli Mose, "Panga njoka na kuifaka pa mutengo. Chizachitika kuti alionse azalumwiwa azapulumuka, akalangana pamene apo." ⁹ Ndipo Mose anapanga njoka ya mukuwa na kuigwilisa ku mutengo. Ndipo njoka ikaluma munthu aliyense, ngati analangana pa njoka ya mukuwa, anapulumuka. ¹⁰ Ndipo banthu baku Israele banayenda ulendo na kupanga misasa mu Oboti. ¹¹ Banayenda kuchoka ku Oboti na kupanga misasa mu Iye Abarimu muchipululu chamene chilangana ku Moabu chaku mumawa. ¹² Kuchokela kuja banayendelela na kumanga misasa mu chigwa cha Zeredi. ¹³ Kuchoka kuja banayendelela na kumanga misasa kumbali ina ya mumana wa Arinoni, wamene uli muchipululu chamene chipitiliza malile ya Aamori. Mumana wa Arinoni upanga malile ya Moabu, pakati pa Moabu na Aamori. ¹⁴ Ndiye chifukwa chake inakamba mu buku ya nkondo ya Yehova, "Waheb mu Sufa, na mu chigwa cha Arinoni, ¹⁵ na kosondomukila kwa zigwa zamene zhipoleka ku muzinda wa Ari na kuyandikizana ku malile ya Moabu." ¹⁶ Kuchoka kuja banayenda ku Beere, pa chisime pamene Yehova anakamba kuli Mose. "Bwelesa banthu bonse pamozi kwa Ine kuti nibapase manzi." ¹⁷ Ndipo Israele anaimba iyi nyimbo: "Tumpula chisime! Imbani pali ichi, ¹⁸ pa chisime chamene basogoleli bathu banakumba, chisime chamene wonveka bana kumba, na ndodo yolamulila. "Kuchokela mu chipululu banayenda to Matana. ¹⁹ Kuchoka ku matana bana yenda ku Nahaliyele, na kuchoka ku Nahaliyele kuyenda ku Bamoti. ²⁰ Na kuchoka ku Bamoti kuyenda ku chigwa mu malo ya Mowabu. Uko ndiye kwamene pa mwamba pa pili ya pisiga kulangana pansu mu chipululu. ²¹ Ndipo Israele anatuma bautenga kuli Sihoni mfumu ya Aamori nakuti, ²² "Lekani tipiteko mukati mu malo yanu. Sitizapatukila mumunda kapena mumunda wampesa. Sitizamwa manzi yamuvisime vanu. Tizapita munjila ya mafumu panka tipitilile mu malile yanu." ²³ Koma Sihoni siinavomeleze Israeli kupitala ku malile yawo. Koma, Sihoni anabwelesa pamozi bankhondo bake nakubanyamukila ba Israeli mu chipululu. Anabwela Jahazi, kwamene anamenyana na Israeli. ²⁴ Israele anabamenya ba nkondo ba Sihoni na lupanga lwakutwa nakutenga malo yawo kuchokela ku Amoni kufikila kukamana Yaboki, kufikila kumalo konse kwa banthu ba Amoni. Ndipo malile ya banthu ba Amoni yanali yolimba. ²⁵ Israeli anatenga mizi zonse za Aamori nakunkalamo monse, kufakilako Hesiboni na minzi zonse. ²⁶ Hesiboni unali munzi wa Sihoni mfumu ya Aamori, bamene banamenyana na mfumu kakudala ya Moabu. Sihoni anatenga yonse malo kuchokela kumalo kwake kufikila ku mumana wa Arinoni. ²⁷ Nichifukwa chake baja bamene bamakamba myambo bamakamba kuti, "Bwelani kwa Hesiboni. Lekani muzi wa Sihoni upangiwenso na kunkazikika futi. ²⁸ Mulilo woyaka kuchoka ku Hesiboni, kupya kwamene kuchokela ku muzi wa Sihoni wamene unawononga Ar wa Moabu, na bene bamalo yapamwamba yaku Arinoni. ²⁹ Nsoni kuli iwe, Moabu! Wawonongeka, banthu ba Kemosi. Apanga bana bake bamuna kunkala wotabataba na bana bake bakazi bankala bakapolo ba Sihoni mfumu ya Aamori. ³⁰ Koma taigonjesa Sihoni. Hesiboni asokonezeka njila yonse kufikila ku Diboni. Tabagonjesa beve njila yonse kufikila ku Nofa, yamene ifika ku Medeba." ³¹ Israele anayamba kunkala mu malo ya Aamori. ³² Ndipo Mose anatuma ba muna kuyenda kuona ku Yazare. Banatenga minzi zawo nakuchosamo ba Aamori benzemo. ³³ Ndipo banapindamuka nakuyenda mu njila yakumwamba ku Basanu. Og mfumu ya Basana anayenda kukubanyamukila, Iye na bonse bankondo bake, kumenyana nawo ku Edreyi. ³⁴ Ndipo Yehova anakamba na Mose, "Usamuyope uyu, chifukwa nakupasa kugonjesa pali eve, bonse bankondo, na malo yake. Chita kuli eve mwamene unachitila kuli Sihoni mfumu ya Aamori, bamene banankalaku Hesiboni." ³⁵ Ndipo banamupaya, bana bake bamuna, ba bese bankondo bake, panka kunalibe banthu bake banasala ba moyo. Banatenga na malo yake.

Chapter 22

¹ Bantu ba Israyele banayenda kufikila pamene banafika nakunkala mu malo ya Mowabu pafupi na Yeliko, kumbali yina ya mumana wa Yodani kuchokela ku muzinda. ² Balaki mwana mwamuna wa Zippori anaona vonse ba Israeli bana chita kwa Aamori. ³ Moabu anayopa bathu chifukwa banali bambili, ndipo Moabu anali na mantha banthu ba Israeli. ⁴ Mfumu yaku Moabu inakamba ku bakulu baku Midian, "Ili gulu bazadya vonse vili muli ife munga mwamene ng'ombe zimadyela mauzu mu munda." Ndipo Balaki mwana mwamuna wa Zippori anali mfumu ya Moabu pantawi ija. ⁵ Anatuma ntumi kuli Balaamu mwana mwamuna wa Beor, pa Pethor yamene ili ku mumana wa Euphrates, mu malo ya ziko yake na bathu bake. Anamuitana na kukamba naye kuti, "Ona, Ziko yabwela kuno kuchokela ku Igupto. Bazulisa malo ya Ziko yapansi ndipo manje bali pafupi naine." ⁶ Napapata bwela manje na kuitembelela iyi ziko mumalo mwanga, chifukwa niwolimba kwaine. Kapena ningakwanise kuyambana nawo na kubachosa muno mumalo. Niziba kuti wamene wadalisa azadaliska, na wamene watembelela azatembелеledwa." ⁷ Koma bakulu ba Moabu na bakulu ba Midian banayenda, notenga chopeleka cha mayele. Banabwela kuli Balaamu na kukamba naye mau ya Balaki. ⁸ Balaamu anabauza kuti, "Nkalani kuno usiku uno. Nizakubweleselani vamene Yehova akamba kuli ine." Ndipo basogoleli ba Moabu banankala na Balaamu usiku uja. ⁹ Mulungu anabwela kuli Balaamu nakuti, "Nibandani aba bamuna babwela kuli iwe?" ¹⁰ Balaamu anamuyanka mulungu, "Balaki mwana wamwamuna wa Zippor, mfumu yaku Moabu, abatuma kwaine. Anakamba, ¹¹ Ona, banthu bamene bachoka ku Igupto vazulisa malo yanga. Koma bwela ndipo ubatembелеle mumalo mwanga. Kapena ningakwanise kumenyana nawo nakubachosa." ¹² Mulungu anamuyanka Balaamu, "Siufunika kuyenda na awo bamuna. Siufunika kutembelela banthu ba Israyele chifukwa banadaliska." ¹³ Balaamu ananyamuka kuseneni nakuuza basogoleli ba Balaki, "Bwelelani ku malo kwanu chifukwa Yehova akana kuti ine niyende naimwe." ¹⁴ Ndipo basogoleli ba Moabu banayenda na kubwelela kuli Balaki. Banakamba, "Balaamu akana kubwela naife." ¹⁵ Balaki anatuma futi basogololi mambili banali wolemekezeka kwambili kuchilila banayenda poyamba. ¹⁶ Banabwela kuli Balaamu nakumuza kuti, "Balaki mwana mwamuna wa Zippori akamba izi, 'napapata leka chinthu chili chonse chisakulese kubwela kuli ine,' ¹⁷ chifukwa nizakulipila bwino maningi nakukupasa ulemu ukulu, ndipo nizachita chilichonse chamene uzaniuzi kuti nichite. Napapata bwela kuti utembelele aba banthu mumalo mwanga." ¹⁸ Balaamu anayankam nakukamba nabamuna ba Balaki, "Olo kapena kuti Balaki anganipase nyumba yake yozula na siliva na golide, siningayende kupitilila mau ya Yehova, Mulungu wanga, nakuchita pan'gono kapena kupitililapo mu vamene aniuza. ¹⁹ manje, yembekezani pano usiku bonse futi, kuti nipunzileko vilivonse vinangu vamene Yehova azakamba naine." ²⁰ Mulungu anabwela kuli Balaamu usiku uja nakukamba kuti, "chifukwa aba banthu babwela kuti bakuitane iwe, nyamuka nakuyenda nawo. Koma uchite chabe chamene nakuuza kuti uchite." ²¹ Balaamu ananyamuka kuseneni, nakukonza bulu wake, na kuyenda nabasogoleli baku Moabu. ²² Koma chifukwa anayenda, Ukulu wamu Mulungu unaonekela. Mungelo wa Yehova anayimilila mu njila munga wina wokulipila Balaamu, wamene anali kuyendela pa bulu wake. Balaamu na banchito bake babili banali naeve. ²³ Bulu anaona mungelo wa Yehova ayimilila pa njila na lupanga mumanja. Balaamu anamenya bulu kuti azibweze munjila. ²⁴ Koma mungelo wa Yehova anaimilila pamalo pang'ono panjila bakati pa munda wa mpesa, na chipupa ku lamanja nachipupa kulamanjele. ²⁵ Bulu anawona mungelo wa Yehova futi. Anayenda nakuzipatikiza kuchipupa na kufwata kwendo kwa Balaamu. Balaamu anaimenya bulu futi. ²⁶ Mungelo wa Yehova anayenda pasogolo na kuimilila pa malo yopatikiza pamene panalibe malo yopindamukila kumbali iliyonse. ²⁷ Bulu anamuona mungelo wa Yehova, ndipo anagona panshi pali Balaamu. Ukali wa Balaamu unanyamuka, na kumenya bulu na ndodo yake. ²⁸ Ndipo Yehova anasegula kamwa ka bulu kuti akambe. Anakamba kuli Balaamu, "Nachita chani kuli iwe kuti ukalipe noyamba kunimenya katatu manje?" ²⁹ Balaamu anayanka bulu kuti, "chifukwa wachita mopusa naine. Ngati ninali na panga mumanja. Ngati inaliko, apa manje sembe nakupaya iwe." ³⁰ Bulu anakamba kuli Balaamu, "Sindine bulu wako wamene umayendelaku masiku ya umoyo wako kufikila nauno usiku? Nilipo navochitika munga vamene vachitika lelo? Balaamu anakamba kuyi, "Iai." ³¹ Ndipo Yehova anasegula menso ya Balaamu, ndipo anamuona mungelo wa Yehova woimilila munjila na lupanga lwakutwa mumanja yake. Balaamu anagwada na kugwesa nkope yake panshi. ³² Mungelo wa Yehova anamuza kuti, "Nichifukwa chani wamenya bulu wako katatu? Ona, nabwela munga wina wokulipa kuli iwe chifukwa vochitika pasogolo panga nivoipa. ³³ Bulu enze aniona nakupindamukila kuchoka kuli ine katatu. ngati senze apindamuka kuchoka kuli ine, sembe nakupaya nakusunga moyo wake." ³⁴ Balaamu anati ku mungelo wa Yehova, "Nachimwa. Sininazibe kuti unaimilila mosusana naine mu njila. Koma manje, ngati sichinakukodwelese iwe, nizabwelela." ³⁵ Koma mungelo wa Yehova anakamba kuli Balaamu, "Yenda pasogolo pamozi namuna. Koma ufunika kukamba chabe mau yamene nizakuza." Mwaichi Balaamu anayenda nabasogoleli ba Balaki. ³⁶ Pamene Balaki ananvela kuti Balaamu abwela,

anayenda panja kuti akumane naye mu muzinda waku Moabu ku Arnoni, wamene uli kumalile. ³⁷ Balaki anati kwa Balaamu, "Sininatume bamuna kuli iwe kuti bakuitane.? Nichani chamene siunabwelele kuli Ine? siningakudalise iwe?" ³⁸ Ndipo Balaamu anamuyanka Balaki, "Ona, nabwela kwaiwe. Ushe manje nili nayo mpavu yokamba chilichonse? Ningakambe chabe mau yamene Mulungu afaka mukamwa mwanga." ³⁹ Balaamu anyenda kwa Balak, ndipo banafika ku Kiriath Huzoth. ⁴⁰ Ndipo Balaki nsembe ya bulu na ng'ombe nakupasa nyama imangu kuli Balaamu na basogololeli banali nayeve. ⁴¹ Kuseni kwake, Balaki anatenga Balaamu pamwamba pa malo ya Baal. Kuchokela kuja Balaamu anakwanisa kuona mbali ina yama Israele mumisasa yawo.

Chapter 23

¹ Balaamu anakamba na Balaki, "Manga ma guwa yali seveni pano yaine na kukonza Ng'ombe zili seveni na mbelele." ² Ndipo Balaki anachita mwamene Balaamu anamuuzila. Ndipo Balaki na Balaamu banapeleka Ng'ombe na Mbelele paguwa lansembe. ³ Ndipo Balaamu kwa Balaki, "Imilila pachopeleka chako cha sembe ndipo nizayenda. Kapena Yehova azabwela kuti tikumane. Chamene azanilangiza nizakuuza." sono anayenda pamwamba pa lupili osatenga mitengo. ⁴ Ndipo Mulungu anamukumyana Balaamu, Ndipo Balaamu anati, "Namanga yali seveni maguwa, na peleka ng'ombe na mbelele paguwa iliyonse." ⁵ Yehova anfaka utenga muli Balamu mukamwa na kuti, "Bwelela kuli Balaki na kukamba nayeve," ⁶ Sono Balaamu anabwelela kuli Balaki, wamene anayimilila pa chopeleka chasembe yake, na bonse wolamulila ba Moabu banali nayeve. ⁷ Ndipo Balaam anayamba kukamba uneneli wake nakuti, "Balaki anileta kuno kuchokela ku Aramu, mfumu ya Moabu kuchokela ku ma pili yaku mumawa. 'Bwela, tembelela Yakobo kwa ine; anakamba. 'Bwela, ononga Israeli. ⁸ Nikatembелеle bwanji bamene Mulungu sana tembelele? Ningasusane nawo banji bamene Yehova sana susane nawo? ⁹ Kuchokela pa mwamba pa mwala namuona; kuchokela pa mapili na mulangana. Ona, kuli banthu bamene bankala ndipo sibazona monga nibanthu bachabe. ¹⁰ Nindani angapende doti ya Yakobo kapena kubelenga chabe wanu-fothi ya Israeli? Lekani ine nife infia ya munthu wolungama, ndipo lekani umoyo wanga usile monga umoyo wake." ¹¹ Balaki anati kuli Balaamu, "Nichani chamene wachita kuli ine? Ninakubweleka kuti utembелеle badani banga, koma ona, wabadalisa." ¹² Balaamu anayanka nakuti, "Sinifunika kunkala ochenjela kumba chabe chamene Yehova afaka mukamwa kanga? ¹³ Koma Balaki anamba naye kuti, "Napapata bwela naine kumalo kwinangu kwamene ungabaone. Uzaonako chabe pafupi naiwo, osati wonse. Kwamene kuja uzabatembelela kwa ine. ¹⁴ Ndipo anatenga Balaamu ku munda wa Zofimu, pamwamba pa pili ya Pisgah, nakumanga ma guwa yali seveni. Anapeleka ng'ombe na mbelele pa guwa iliyonse. ¹⁵ Koma Balaamu anauza Balaki kuti, imilila pano pa zansembe zako, pamene nikumana na Yehovah kuja kusogolo." ¹⁶ Ndipo Yehova anakumana na Balaamu na kuika utenga mukamwa kake. Anakamba kuti, ¹⁷ "Balaamu bwelela kuli eve, na Kuona, enze aimilila ba guwa ya nsembe yake, nabasogoleli ba Moabu banali nayeve. Koma Balaki anakamba naye kuti, "Nivichani vamene Yehova akamba?" ¹⁸ Balaamu anayamba kunenela. anakamba kuti, "Nyamuka, Balaki, na kunvela. Nvela kwaine, Iwe mwana mwamuna wa Zippori. ¹⁹ Mulungu simunthu, kuti anganame, kapena munthu, kuti angachinje nzeru zake. Ushe analonjezapo chilichonse nokana kuchichita? Anakambapo kuti nizachita chinthu nokana kuchisebenzelapo? ²⁰ Onani, nakuuzidwa kudalisa. Mulungu apasa daliso, ndipo siningaibweze. ²¹ Sanalangapo kuvutika mu Yakobo, ndipo sanaonepo mazunzo mu Israeli. Yehova Mulungu wabo alinawo, na kukamba kwa mfumu kuli pakati pawo. ²² Mulungu anabachosa mu Igupto na mpavu monga nyama yamusanga. ²³ Kulibe mfuti yamene isebenza mosusana na Yakobo, kulibe na wonenela vaboza bazawononga Israel. mwaichi, chizakambidwa pali Yakobo na Israeli, 'Ona vamene Mulungu achita!' ²⁴ Onani, banthu banyamuka monga nkalamu zikazi, mwanene nkalamu imabendelela na kuononga. siimagona pansi panja idye wamene yagwila na kumwa magari ya chamene yapaya." ²⁶ Koma Balaki anati kwa Balaamu, "Usabatembelele kapena kubadalisa. ²⁵ "Koma Balaamu anayanka na kuti kuli Balaki, "Sininakuuze kuti nifunika kukamba vonse vamene Yehova aniuza kuti nikambe?" ²⁷ Koma Balaki ayanka Balaamu, "Bwela manje, nizakupeleka ku malo yenangu. Kapena chizakondweleka Mulungu kuti iwe ubatembele kwamene kuja kwa Ine." ²⁸ Ndipo Balaki anatenga Balaamu pa mwamba pa lupili lwa Peor, lwamene lulangana pansu mu chipululu. ²⁹ Balaamu anati kuli Balaki, "Nimangile ma guwa yali seveni pano na ng'ombe zili seveni na mbelele zili seveni." ³⁰ Ndipo Balaki anachita mwamene Balaamu anamuuzila, anapeleka nsembe ya ng'ombe na mbelele pa guwa iliyonse.

Chapter 24

¹ Pamene Balaam anaona kuti chinakondwelesa Yehova kudalisa Israeli, sanayende, monga ntawi zinangu, kusebenjesa majiki. Mwaichi, analangana pasogolo pa chipululu. ^{2 3} Ananyamula menso yake na kuona kuti Israeli anakamping'a, aliyense pamutundu wake, na Muzimu wa Mulungu unabwela pali eve. Analandila uyu uneneli na kuti, "Balaamu mwana mwamuna wa Beor ali pafupi nakukamba, munthu wamene menso yake niyoseguka maningi. ^{4 5} Amakamba na kunvela mau ya Mulungu. Amaona masopenya kuchokela kwa Yehova, pambuyo pake amagwada pansi namenso yake yoseguka. Niyambwino ma tenti yanu, Yakobo, malo yamene munkalamo, Israeli! ⁶ Monga vigwa batambalala, monga minda mumbali mwa mimana, monga aloye zoshangiwa na Yehova, monga mikunguza zamumbali ya manzi. ⁷ Manzi yazapaka kuchokela mu mabaketi yawo, na mbeu zawo zizankala na yambili manzi. Mfumu yawo izankala yochuka kupitilila Agag, na na ufumu waka uzalemekezeka. ⁸ Mulungu azmuchosa mu Igupto. Azankala na mpavu monga nyama ya musanga. Azayandwa maziko yamene yazafuna kumuukila. Azapwanya ma bonzo yawo muviduswa. Azaba shuta na mivu yake. ⁹ Anakalaba pansi monga nkalamu, monga nkalmu ikazi. Nindani angafunine kumuyamba? Lekani wamene afuna kumudalisa adalisike; lekani wamene afuna kumutembelela atembeledwe." ¹⁰ Balaki bukali wake unakula mosusana na Balaamu na kumenya manja yake pamozi mu ukali. Balaki anakamba kuli Balaamu kuti, "Ninakuitana kuti utembelele badani banga, koma ona, wabadalisa katatu. ¹¹ Sopano nisiye manje ndipo yenda kunyumba. Ninakuuza kuti nizakudalisa iwe, koma Yehova akusunga iwe kuti usatenge iliyonse daliso." ¹² Ndipo Balaamu anamuyanka Balaki, "Ninakamba nawo batumiki bamene unatuma kuli ine, ¹³ Ngankale kuti Balaki ananipasa ine nyumba yake yozula na siliva na golide, siningayende mosusana na mau ya Yehova na vilivonse voipa kapena vabwino, kapena vilivonse kuli vonse vamene ningafune kuchita. Ningakambe chabe vamene Yahova aniuza ine kukamba.' ushe sininauze ivi? ¹⁴ Koma manje, ona, nizayenda kubanthu banga. Koma choyamba leka nikuzibise vamene aba banthu bazachita kubanthu bako mumasiku yobwela." ¹⁵ Balaamu anayamba kunenela. Anakamba, "Balaamu mwana mwamuna wa Beor akamba, mwamuna wamene menso yake niyoseguka maningi. ¹⁶ Uyu niuneneli wa munthu aliwonse wamene akunva mau kuchokela kwa Mulungu, ali nanzelu kuchochola kwa Wamumwa, wamene amaona kuchokela ku wampavuzonse, pasogolo pa wamene iye amagwadila pansi na menso yoseguka. ¹⁷ Namuona, koma salipo pano manje. Nimulangana, koma sali pafupi. Nyenyezi izabwelela kuchoka muli Yakobo, naulamulilo uzanyamukila kuchoka mu Israeli. Azazizilika basogoleli ba Moabu na kuwonenga bonse bamubadwe wa Seti. ¹⁸ Koma Edomu azankala malo ya Israele, na Seir azankalanso malo yawo, badani ba Israele, bamene Israeli azagonjesa mwa mpavu. ¹⁹ Kuchokela muli Yakobo mfumu izabwela wamene azankala na ulamulilo, ndipo azaononga wosalapo mu muzinda." ²⁰ Ndipo Balaamu anayangana kuli Amaleki na kuyamba uneneli. Anakamba kuti, "Amaleki anali pantawi inangu ziko youchuka, koma kusiliza kwake chizankala chionengeko." ²¹ Ndipo Balaamu analangana pasogogolo pa Kenites na kuyamba uneneli wake. anakamba, "Malo yamene munkalamo niyokosa, na vinsa vanu mummyala. ²² Ngankaleso iwe ba Kenites mu zapyia na mulilo pamene ma Assiriya bakakutengani mu ukapolo." ²³ Ndipo Balaamu anayamba uneneli wake wosiliza. Anakamba, "Tembelelo! Ndani azpulumuka pamene Mulungu akachita ichi? ²⁴ Ma shipu yazabwela kuchoka ku nyanja ya Kittimu; bazamenyana ndi Assiriya na kugonjesa Eber, koma nabeve, bazasilizila mu chionengeko." ²⁵ Ndipo Balaamu ananyamuka na kuyenda. Anabwelela kunyumba kwake, na Balaki naye anayenda.

Chapter 25

¹ Israeli anankala mu Shittimu, na bamuna banayamba ubule beve nabakazi baku Moabu, ² chifukwa ma Moabi banabaitana banthu ku chosepeleka chancebe ku milungu yawo. Ndipo banthu banadya na kugwadila pansi milungu yama Moabi. ³ Bamuna ba Israeli banasankinizika muku lambila Baala waku Peor, na Yehova ukali wake unanyamuka kususana na Israeli. ⁴ Yehova anakamba na Mose, "Paya bonse basogoleli ba banthu na kubapachika pamwaba pamenso panga kuti baonekele mu zuba, kuti ukali wanga uchekepo pali Israeli." ⁵ Ndipo Mose anati kwa basogoleli ba Israeli, "Aliwonse wa inu afuka kupaya banthu bake bamene banasankanizika mukuyamika Baal waku Peor." ⁶ Ndipo umozi wa mwamuna wa bana bamuna ba Israeli anabwela na kuleta mwa ba banja bake mumukazi waku Midianiti. Ichi chinachitika pamenso pa Mose na bonse ba munzi wa banthu ba Israeli, pamene banali kulila pongenela pa tenti yokumanilamo. ⁷ Pamene Finihasi mwana mwamuna wa Eleazar mwana mwamuna wa Aaroni woipepeka chansebe, anaona chija, ananyamuka kuchokela pakati pa munzi nakutenga lupanga mumanja mwake. ⁸ Anakonka mwamuna wa Israeli mu tenti na kujuba lupanga kupita muli bonse mumatupi yawo, bonse mwamuna wa Israeli na mukazi. kuti chilango chamene Mulungu anatuma pa banthu ba Israeli chileke. ⁹ Awo banafa na lupanga banali twenti-folo sauzande munamba. ¹⁰ Yehova anakamba na Mose na kuti, ¹¹ "Finiyasi mwana mwamuna wa Eleazar mwana mwamuna wa Aaroni woipeleka nsembe, apindamula ukali wanga kuchoka pa banthu ba Israeli chifunaka anali nachocho chifundo nakuponyako nzelu pakati pawo. Ndipo sininaonenge banthu ba Israeli mu ukali wanga. ¹² Ndiponso kamba, 'Yehova akuti, 'Ona, Nizapasa Finiyasi chipangano chamutendele. ¹³ Kuli iye na kumibadwe izambwela pa mbuyo pake, chizankala chipangano chamuyaya cha opeleka nsembe chifuka anali wolimba pali ine, Mulungu wake. Azilangina pa bathu ba Israeli.'" ¹⁴ Manje zina ya mwamuna waku Israeli wamene anapayiwa pamozi mukazi waku Midianiti anali Zimuri mwana mwamuna wa Salu, musogoleli wa makolo mubanja muli Simeonites. ¹⁵ Zina ya mukazi waku Midianite wamene anapayiwa inali Kozbi mwana mukazi wa Zur, wamene anali mukulu wa mutundu na banja mu Midiani. ¹⁶ Ndipo Yehova anakamba kuli Mose na kuti, ¹⁷ Ubasunge ma Midianiti monga badani nakumenyana nayo, ¹⁸ chifukwa banakusungani onga badani na ukuluku wawo. Banakupelekani imwe mu uchimo in mulandu wa Peor na mumulandu wa mulongo wawo Kozbi, mwana mukazi wa musogoleli ku Midian, wamene anapayiwa pa siku la chilango mu vintu va Peor."

Chapter 26

¹ Kunabwela kuti patapita chilango kuti Yehova anakamba na Mose na Eleazar mwana mwamuna wa Aaroni wopeleka wansembe. Anati, ² "Belangani bonse mumunzi banthu ba Israeli, kuchoka pa zaka zili twenti na kuyenda pamwamba, kupitila mukubadwa kwa makola yawo mubanja, bamene bangayende kunkondo mumalo mwa Israeli. ³ Sopano Mose na Eleazar wopwleka nsembe banakamba nabeve in mu malo ya Moabu mu Yodaniku Yeriko na kuti, ⁴ Belenga banthu, kuchokela pa zaka twenti na pamwamba, mwamene Yehova auzila Mose na banthu ba Israeli, banachoka mu ziko ya Igupto." ⁵ Rubeni anali mwana woyamba wa Israeli. Kuchokela ku mwana wake wamwamuna kunabwela mutundu waba Hanokites. Kuchoka Pallu kanabwela mutundu wa ba Palluites. ⁶ Kuchoka Hezroni kunabwela mutundu wa ba Hezronites. Kuchoka Karmi kunabwela mutundu wa ba Karmites. ⁷ Uyu ndiye mubadwe wa Reubeni, unabelengedwa 43, 730 bamuna. ⁸ Eliabu anali mwanza mwamuna wa Pallu. ⁹ Eliabu bana bake bamuna banali Nemuel, Dathan, na Abiramu. Aba ndiye banali bamozi Dathan na Abiramu banakonka Korah pamene banakangana na Mose na Aaroni nakusanvelela Yehova. ¹⁰ Ziko yapansi inasegula kamwa kake nakubamela bonse pamozi na Korah pamene bomukonka banafa. Pantawi ija, mulilo unashoka 250 bamuna, bankala chisanzo. ¹¹ Koma banali mumuzela wa Korah sibanafe panja. ¹² Mubadwe wa Simeon's bana bake banali aba: Kupitila muli Nemuel, mubadwe wa Nemuelites, kupitila muli Jamini, mubadwe wa ba Jaminites, kutila muli Jakin, mubadwe waba Jakinites, ¹³ kupitila muli Zerah, mubadwe waba Zerahites, kupitila muli Shaul, mubadwe waba Shaulites. ¹⁴ Iyi inali mibadwe ya bobadwa muli Simeon, banapendewa 22,200 bamuna. ¹⁵ Mibadwe ya bana ba Gadi ni iyi: kupitila muli Zephoni, mubadwe wa ba Zephonites, kupitila muli Haggi, mubadwe wa ba Haggites, kupitila muli Shuni, mubadwe waba Shunites, ¹⁶ kupitila muli Ozni, mubadwe waba Oznites, kupitila muli Eri, mubadwe waba Arites, ¹⁷ kupitila muli Arod, mubadwe waba Arodites, kupitila muli Areli, mubadwe waba Arelites. ¹⁸ Iyi ndiye mibadwe ya bana ba Gadi, banabelengedwa 40, 500 ba muna. ¹⁹ Bana bamuna ba Yuda banali Er na Onan, koma aba bamuna banafa mu malo ya Kanani. ²⁰ Mubadwe wa Yuda nabana bake benangu banali aba: Kupitila muli Shelah, mubadwe waba Shelanites, through Perez, mubadwe wa Perezites, na kupitila muli Zerah, mubadwe wa Zerahites. ²¹ Bana ba Perez banali aba: Kupitila muli Hezroni, mubadwe waba Hezronites, kupitila muli Hamul, mubadwe waba Hamulites. ²² Iyi ndiye mibadwe ya bana ba Judah, banabelengedwa 76, 500 bamuna. ²³ Mibadwe za Issacha nabana bake benze aba: Kupitila muli Tola, mubadwe waba Tolaites, kupitila muli Puah, mubadwe waba Puites, ²⁴ kupitila muli Jashub, mubadwe waba Jashubites, kupitila muli Shimron, mubadwe waba Shimronites. ²⁵ Iyi ndiyo inali mibadwe ya Issachar, banabelengedwa 64,300. ²⁶ ²⁷ Mubandwe wa Zebuluni na bana bake inali iyi: Kupitila muli Saredi, mubadwe waba Seredites, kupitila muli Elon, mubadwe waba Elonites, kupitila muli Jahleel, mubadwe waba Jahleelites. Iyu ndiwo unali mubadwe wa Zebulunites, banabelengedwa 60,500 bamuna. ²⁸ Mubadwe wa bana ba Yosefe banali Manasseh na Ephraim. ²⁹ Bana ba Manasseh banali aba: kupitila muli Makir, mubadwe waba Makirites (Makir anali tate wa Gilead), kupitila muli Gilead, mubadwe waba Gileadites. ³⁰ Bana ba Gileadi banali aba: Kupitila muli Lezer, mubadwe waba Lezerites, kupitila muli Helek, mubadwe waba Helekites, ³¹ kupitila muli Asriel, mubadwe waba Asrielites, kupitila muli Shechem, mubadwe waba Shechemites, ³² kupitila muli Shemida, mubadwe waba Shemidaites, kupitila muli Hephher, mubadwe waba Hephherites. ³³ Zelophehad mwana mwamuna wa Hephher analibe bana bamuna, koma chabe bana bakazi. Mazina ya bana bakazi yanali Mahlah, Noah, Hoglah, Milkah, na Tirzah. ³⁴ Iyi inali mibadwe ya Manasseh, inabelengedwa 52, 700 bamuna. ³⁵ Mibadwe ya bana ba Ephraim inali iyi: Kupitila muli Shethelah, mubadwe waba Shuthelaties, kupitila muli Beker, mubadwe waba Bekerites, kupitila muli Tahan, mubadwe waba Tahanites. ³⁶ Wobadwa kuli Shuthelah banali, Eran, mubadwe waba Eranites. ³⁷ Uyu ndiwo unali mubadwe wa Ephraimu mubana bake, banabelengeka 32, 500 bamuna. Aba banali wobandwa mwa Yosefe, banapendewa mwa mutundu wa mubadwe wawo. ³⁸ Mubadwe wa Benjamini mu bana bake banali aba: Kupitila muli Bela, mubadwe wa Belaites, kupitila muli Ashbel, mubadwe wa Ashbelites, kupitila muli Ahiramu, mubadwe waba Ahiramites, ³⁹ kupitila muli Shuphamites, kupitila muli Hupham, mubadwe waba Huphamites. ⁴⁰ Bana ba Bela banali Ard na Naaman. Kuchokela kuli Ard kunabwela mubadwe waba Ardites, na kuchokela kuli Naaman kunabwela mubadwe waba Naamites. ⁴¹ Uyu ndiwo mubadwe ya Benjamin mu bana bake. Bana pendewa 45, 600 bamuna. ⁴² Mubadwe wa Dan mu mubadwe banali, Kuli Shuham, mubadwe waba Shuhamites. ⁴³ Aba banali Mubadwe wa Shuhamites banabelengedwa 64, 400 bamuna. ⁴⁴ Mubadwe wa Asher mukubadwa inali iyi: Kupitila muli Imnah, mubadwe waba Imnites, kupitila muli Ishvi, mubadwe waba Ishvites, kupitila muli Beriah, mubadwe waba Beriites. ⁴⁵ Bana ba Beriah banali aba: Kupitila muli Heber, mubadwe waba Heberites, kupitila muli Malkiel, mubadwe waba Malkielites. ⁴⁶ Zina ya mwana mukazi wa Ashe anali Serah. ⁴⁷ Iyi inali mibadwe ya Asher mubana bake, banabelengedwa 53, 400 bamuna. ⁴⁸ Mibadwe ya Naphtali mukubadwa inali iyi: Kupitila muli Jahzeel, mubadwe waba Jehzeelites, kupitila muli Guni, mubadwe waba Gunites, ⁴⁹ kupitila muli

Jezer, mubadwe waba Jezerites, kupitila muli Shillem, mubadwe waba Shillemites.⁵⁰ Iyi inali mibadwe ya Naphtali mukubadwa, banabelengeka 45,400 bamuna.⁵¹ Iyi inali yokwanila mabelengedwe ya ba muna ba Israeli: 601,730.⁵² Yehova anakamba na Mose na kuti,⁵³ "Malo yafunika kuyagabanisa mukati mwa aba bamuna monga chopasiwa mwamene namba ilili mumazina yawo.⁵⁴ Ku ikulu mibadwe ufunika kuipasa yambili gawo, na mibadwe ing'ono ufinika kuipasa ing'ono gawo. Ku banja iliyonse ufunika kuipasa gawo mwanene balili namba yabamuna bamene banabelengedwa.⁵⁵ Mwaichi, malo yafunika kugabikana mwazizizi mochaya mayele. Bafunika kutenga malo mwamene yazagabikila mwaneme ilili mitundu ya makolo yawo.⁵⁶ Magwo yawo yafunika kugabanisa mu ukulu na muung'ono mubadwe. kupasidwa kuli beve mwazizizi mukuchaya mayele."⁵⁷ Mibadwe za ba Levite, yopendewa mudadwe pa mubadwe, zinali izi: kupitila muli Gershoni, mubadwe waba Gershonites, kupitila muli Kahath, mubadwe waba Kohathites, kupitila muli Merari, mubadwe waba Merarites.⁵⁸ mubadwe wa Levi unali uyu: mubadwe waba Libnites, mubadwe waba Hebronites, mubadwe waba Mahlites, mubadwe waba Mushites, na mubadwe waba Korahites. Kohath anali chikolwe cha Amuramu.⁵⁹ Zina ya mukazi wa Amuramu anali Jochebedi, wobadwa muli Levi, wamene anabadwa kwa Levite mu Egipto. Anabla kwa Amuramu bana bawo, bamene banali Aaron, Mose, na Miriamu kalongosi yawo.⁶⁰ Kuli Aaroni kunabadwa Nadabu na Abihu, Eleazar na Ithamar.⁶¹ Nadabu na Abihu banafa pamene banapeleka kwa Yehova osayenela mulilo.⁶² Bamuna banabelengedwa pamozi mabelengelo twenti-fili sausand, bonse bamuna kuyambila pa mwezi umozi kuyenda pamwamba. Koma sibanabelengedwe pamozi na bobadwa mwa Israeli chifukwa kuli gawo inapasidwa kuli beve pamodzi na banthu ba Israele.⁶³ Aba ndiwo bamene bana belengedwa na Mose na Eleaza wopeleka nsembe. Banabelenga banthu ba Israele in sanga ya Moabu pa Yodani mu Yeriko.⁶⁴ Koma mwa aba kunalibe mwamuna wamene anabelengedwa kuli Mose na Aaroni wopeleka nsembe pamene wobadwa ba Israele banabelengedwa muchipululu cha Sinayi.⁶⁵ Chifukwa Yehovah anakamba kuti bonse awo banthu bazafela mu chipululu. Munalibe munthu anasala mukati mwawo, kunasala chabe kalebu mwana mwamuna wa Jephunneh and Joshua mwana mwamuna wa Nun.

Chapter 27

¹ Ndipo kwa Mose kunablwela bana bakazi ba Zelophehad mwana mwamuna wa Hepher mwana mwamuna wa Gileadi mwana mwamuna wa Makir mwana mwamuna wa Manasseh, wa mubadwe wa Manasseh mwana mwamuna wa Yosefe. Aya ndiyo yanali mazina ya bana bake bakazi: Mahlah, Noah, Hoglah, Milkah, na Tirzah. ² Banaimilila pa sogolo pa Mose, Eleazar wopeleka nsembe, ba sogoleli, na basogolo pa bonse mumunzi pongenela mu tenti yokumanilamo. Nanati, ³ "Batate bathu banafa muchipululu. Sibanali pamozi na awo bananvelana kusunsana na Yehova mu kugwiliza na Korah. Banafa chifukwa cha uchimo wawo, ndipo banalibe bana bamuna. ⁴ Nichifukwa chani zina ya batate bathu ichokepo pakati pa banthu ba mubadwe chifukwa banalibe mwana mwamuna? Tipaseni malo pakati pa babululu baba Tate." ⁵ Sono Mose anabwelesa mulandu wawo pasogolo pa Yehova. ⁶ Yehova anakamba na Mose na kuti, ⁷ "Bana bakazi ba Zelophehad bakamba chilungamo. Mufunika kubapasa malo monga gawo pamozi na banja yaba tate bawo, na kuonesesa kuti gawo ya batate bawo ipite bali beve. ⁸ Ufunika kukamba na banthu ba Israele na kuti, 'Ngati mwamuna afa ndipo alibe mwana mwamuna, ufunika kupanga kuti gawo yake izipita kubana bake bakazi. ⁹ Ngati alibe mwana mukazi, mwaichi mufunika kapasa gawo yake kuli ba bale bake. ¹⁰ Ngati alibe ba bale bake, mwaichi mufunika kupasa gawo yake kuli ba bale baba tate bake. ¹¹ Ngati batate bake balibe ba bale, mufunika kupasa gawo yake kuba pafupi ba banja mumibadwe yake, ndipo afunika kuzitengela pa yeka. Iyi izankala lamulo yoikidwa mukukamba ku banthu ba Israele, monga Yehova alamulila ine.'" ¹² Yawe anakamba na Mose, "Yenda pamwamba pa mapili ya Abarim na kuona pa malo yamene napasa banthu ba Israele. ¹³ Pambuyo pake ukayaona, you, naiwe, mufunika kusonkana ku banthu bako, monga Aaroni mubale wako. ¹⁴ Ichi chizachitika chifukwa imwe babili munashushana nakuukila malamulo yanga mu chipululu cha Zini. Kuja, pamene manzi yanachoka mu mwala, muukali wanu munakangiwa kulemekeza Ine monga woyela basogolo pa menso ya munzi wonse." Aya nimanzi ya Meribah ya Kadesh muchipilulu cha Zini. ¹⁵ Ndipo Mose anakamba na Yehova na kuti, ¹⁶ "Lekani Imwe, Yehova, Mulungu wa mizimu za bonse muntu, sankani mwamuna pamwamba pa munzi, ¹⁷ mwamuna wamene angayende panja na kubwela mukati basogolo yawo na kubasogolela kuyenda panja nakubwela nawo mukati, kuti munzi wanu usankale monga mbelele yamene ilibe kachema." ¹⁸ Yehova anati kwa Mose, "Tenga Yoshua mwana mwamuna wa Nun, mwamuna muli yeve mwamene muzimu wanga unkala, ndipo utambalike kwanja kwako pali yeve. ¹⁹ Mubwelese basogolo pa Eleazar wopeleka nsembe na pasogolo pa bonse bamumunzi, na kumuza iye basogolo pa menso yawo kuti abasogolele. ²⁰ Ufunika kuika winangu ulamulilo pali yeve, kuti bonse munzi wa banthu ba Israele bazimunvelela iye. ²¹ Azayenda pasogolo pa Eleazar wopeleka nsembe mukufuna chifunilo changa pali yeve mu makanizo ya Urimu. Izankala pali yeve kukamba kuti banthu bazayenda panga nakubwela mukati, bonse yeve na banthu ba Israele naeve, na munzi wonse." ²² Ndipo Mose anachita monga mwamene Yehova anamuuzila iye. Anatenga Joshua na kumufaka iye pasogolo pa Eleazar wopeleka nsembe na wonse munzi. ²³ anatambalika manja yake pali yeve naku muza yeve kuti asogolele, mwamene Yehova anakambila kuti iye achite.

Chapter 28

¹⁶ Ninalamulila boweluza banu pa ntau ija, kukamba, 'Nvelani mikangano pali ba bale banu, nakuweluza molungama pakati muntu na mubalae wake, na mulendo wamene ali naye. ¹⁷ Imwe simufunika kulangiza kusanka ku aliyense ali mu kususana; imwe muzanvela mung'ono na wonveka molingana. Imwe simuzayopa maonekedwe ya mwamuna, chifukwa chiweluzo nicha Mulungu. Kususana kwamene kuli kovuta kuli imwe, muzambwelesa kwaine, ndipo ine nizanvela. ¹⁸ Nikulamulilani pali ija ntawi vinthu vonse vamene mufunika kuchita. ¹⁹ Tinayenda kuchoka ku Horeb na kuyenda mukati monse mwa monveka na moyofya muchipululu chamene munaona, munjila yathu ku ziko yapapili ya Amori, monga Yehova Mulungu wathu anakambila; ndipo tinabwela ku Kadeshi Barbea. ²⁰ Ine ninakamba naimwe, 'Mufunika kubwela ku lupili ya ziko ya Amori, yamene Yehova Mulungu wathu atipasa. ²¹ Onani, Yehova Mulungu wanu aika malo pasogogolo panu; yendani pamwamba, tengani malo, monga Yehova, Mulungu wa batate banu, akambila kwa imwe; simufunika kuyopa, kapena kunkala wokumudwa. ²² Aliyense pali imwe anabwela kuli ine nakukamba, 'tiyeni titume bamuna pasogolo patu, kuti banga tioneleko malo, nakutiletela mau mwamene tikamenyele nkondo, na mizinda yamene tizangenamo. ²³ Nkani iyi inanikondwelesa maningi; ninatenga bamuna tveovu pali imwe, mwamuna umozi kuchoka kumutundu uli onse. ²⁴ Banabwela naku yenda kuziko yaku mapili, banabwela ku chikwa cha Eshikoli, naku ona ona. ²⁵ Banatenga vina vipaso vamu ntaka mu manja mwawo nakuleta kuli ife. Banabwelensanso kwa ife mau na kuti, 'Ni malo yabwino yamene Yehova wathu Mulungu atipasa. ²⁶ Koma munakana kuukila, koma muna pandukila mosusana na malamulo ya Yehova Mulungu wanu. ²⁷ Munadandaula mu misasa yanu na kuti, 'Ni chifukwa kuti Yehova anatizonda ife kuti Iye abwelesa kwife kuchoka mu malo ya Igupto, kutipasa mukati mumanja ya Amori kutiononga ife. ²⁸ Nikuti kwamene tinga yende manje? Bathu babale bapanga yathu mitima kusungunika, kuti, 'Awo bathu ni bakulu na batali kuchila mwamene tilili; Minzi yawo ni ikulu ndipo niyolimba kufika kumwamba; koma, tababona bana bamuna ba Anakimu kuja.' ²⁹ Ndipo ninakamba kuli imwe, 'Musankale na manta, kapena musayope beve. ³⁰ Yehova Mulungu wanu, wamene ayenda pasogolo panu, azakumenyelani, monga vilivonse vamene anachita kuli imwe mu Igupto pamenso panu, ³¹ na futi muchipululu, kwamene munaona mwamene Yehova Mulungu wanu anakutengelani, monga mwamuna atengela mwana wake mwamuna, kulikonse kwamene munayenda kufikila munabwela kuli yano malo.' ³² Koma ngankale aya mau simunakulupilile Yehova mulungu wanu, ³³ analikuyenda pasogolo panu kukupezelani malo imwe yapangilapo musonkano, mumulilo usiku na mukumbi muzuba. ³⁴ Yehova ananvela chongo cha mau yanu na kukalipa; analapa na kuti, ³⁵ 'Zoona kulibe umozi wa aba bamuna bauyu mubadwe wochimwa uzaona yabwino malo yamene ninalumbila kupasa makolo yanu, ³⁶ kuchosako Kalebu mwana mwamuna wa Jephunneh. Azaiona ndipo nizamupasa iye na wobadwa mumalo yamene anadyakamo, chifukwa anamukonka Yehova.' ³⁷ Komanso Yehova anali wokalipa naine chifukwa cha imwe, nakuti, 'Naiwe siuzayenda kuja; ³⁸ Yoswa mwana mwamuna wa Nuni, wamene aimilila pasogolo panu, azayenda kuja; mulimbikiseni, chifukwa azasogolela Israeli kuti batenge malo. <<<<<<< HEAD ³⁹ Komanso, bana banu bang'ono, bamene munakamba kuti bazankala wozunzika, bamene lelo balibe nzelu za bwino kapena zoipa - bazayenda kuja. Kuli beve nizabapasa, ndipo bazatenga kunkala yawo. ⁴⁰ Koma imwe, pindamukani na kutenga ulendo wanu mu chipululu kupitila mu njila yaku nyanja ya Reedis.' ===== ³⁹ Elo, bana banu bang'ono, bamene munakamba kuti baza vutikilamo, bamene lelo balibe nzelu zoziba chabwino na choipa-bayenda kungeni muja. Kuli beve nizaba pasa, ndipo yazankala yao. ⁴⁰ Koma kwaimwe, pindamukani nakuyambako ulendo wanu muchipululu mubali mwanjila yaku mumana wa Reedi.' >>>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 <<<<<<< HEAD ⁴¹ Ndipo munaniyanka na kuti, 'Tachimwa mosusana na Yehova; tizayenda na kumenyana, ndipo tizakonka vonse vamene Yehova Mulungu wathu atilamulila ife kuti tichite.' Aliyense mwamuna muli imwe avale zida zake zankondo, ndipo munali okonzeka ku gonjesa ziko yapapili. ⁴² Yehova anakamba kuli ine, 'Kamba kuli beve, 'musaukile na osamenya, chifukwa sinizankala na imwe, ndipo muzagonjesedwa kuli badani banu.' ===== ⁴¹ Mwaicho muna yanka nakukamba kuli ine, 'Tachimwila Yehova; tizayenda nakumenya bantu bamumalo yaja, ndipo tizakonka vonse vamene Yehova mulungu watu alamulila ife kuchita.' Mwamuna aliyense pali imwe avale chida chake cha nkondo, mwaicho munali bkonzeka kumenya ziko yaku mapili. ⁴² Yehova anakamba kuli ine, 'kamba kuli beve, 'Musachite ndeo kuli aba bantu nakubamenya, chifukwa sinizankala na imwe, mwaicho muzamenyewa naba dani banu.' >>>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 ⁴³ Ninakamba kuli imwe muli iyi njila, koma simunanvele. Munapanduka mosusana na malamulo ya Jehova; Munali ozikuza na kuukila ziko yapapili. ⁴⁴ Koma ma Amori, bamene banankala pa ziko yapapili, banabwela mosusana naimwe na kukupilikishani monga nzimu, na kumenya imwe pansu mu Seir, kutali monga ku Hormah. <<<<<<< HEAD ⁴⁵ Munabwela na kulilila pamenso pa Yehova; Koma Yehova sananvele ku mau yanu, kapena kuponyako nzelu kuli imwe. ⁴⁶ Ndipo munankala mu Kadeshi masiku yambili, yonse masiku yamene munankala kuja. ===== ⁴⁵ Munabwelela naku lila pamenso pa Yehova; koma Yehova sananvele mau yanu, olo kuikilako nzelu kuli imwe. ⁴⁶ Mwaicho munankala ku Kadeshi masiku yambili, yonse masiku yamene munankala kuja. >>>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84

Chapter 2

¹ Mwaicho tinabwelela nakuyambako ulendo watu muchipululu munjila yaku mumana wa Reedi, monga mwamene ² Yehova anakambila kuli ine; tinayenda mozunguluka pili ya Seiri masiku yambili. Yehova anakamba kuli ine, kukamba, ³ mwayenda mozunguluka pili iyi ntau itali; konekelani kumalo yaku mpoto. >>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 <<<<<< HEAD ⁴ Bauze banthu, nakuti, "Mufunika kupita mukati mwa boda ya babale banu, bana ba Esau, bamene bankala mu Seir; bazakuyopani imwe. Koma munkale osamala ⁵ musayese kumenyana nawo, chifukwa sinizakupasani yaliyonse malo yawo, iyai, ngankale kapena yokwanila kwendo imozi kudyakamo; chifukwa napasa pili ya Seir kuli Esau kukala nayo. ===== ⁴ Lamula bantu, kamba, "Mufunika kupita mumalile yaba bale banu, mubadwe wa Esau, bamene bankala mu Seiri; bazakuyopani. Mwaicho nkalani bochenjela ⁵ kuti musamenyane nabo, chifukwa sinizakupasani malo yali yonse yao, iyai, osati ngankale kang'ono pamalo yao kodyakapo; chifukwa napasa pili ya Seiri kuli Esau kunkala chintu chake. >>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 <<<<<< HEAD ⁶ Muzagula vakudya kuchoka kuli beve na ndalama, kuti mudyey; ndiponso muzagulanso manzi kuchoka kuli beve na ndalama, kuti mumwe. ⁷ Chifukwa Yehova Mulungu wanu akudalisani imwe mu zonse nchito zanu zamanja; Aziba kuyenda kwanu kupita mu chipululu chachikulu. Muli izi zaka zili fote Yehova Mulungu wanu ankala naimwe, ndipo simunasobe kalikonse." ===== ⁶ Muzagula vakudya kuli beve pa ndalama, kuti mungadye; muzagula na manzi kuli beve pa ndalama, kuti mungamwe. ⁷ Chifukwa Yehova mulungu wanu akudalisani munchito iliyonse ya manja yanu; aziba kuyenda kwanu kupita muchipululu chikulu. Kwa izi zaka fote Yehova mulungu wanu anali na imwe, ndipo simunasobe kali konse." >>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 <<<<<< HEAD ⁸ Ndipo tinapita kuli ba bale bathu, bana ba Esau bamene bankala ku Seir, kutali kuchoka ku museu wa Arabah, kuchoka ku Elath na kuchoka ku Ezion Geber. Ndipo tinapindimuka na kupita ku njila muchipululu cha Moabu. ===== ⁸ Mwaicho tinapita kuli ba bale batu, mubadwe wa Esau banali kunkala ku Seiri, kutali na njila yaku Araba, kuchokela ku Elati naku Ezioni Gebe. Mwaicho tina koneka naku pita mu njila yaku chipululu chaku Moabu. >>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 <<<<<< HEAD ⁹ Yehova anakamba na ine, 'Usamuvutise Moabu, ndipo osayese kumenyana nawo mu nkondo. Chifukwa sinizakupasa yake malo kuti unkale nayo, chifukwa napasa Ar kuli bana ba Loti, kuti yankale yawo.' ===== ⁹ Yehova anakamba kuli ine, 'osati kuvuta Moabu, nakusamenyana nabo mu nkondo. Chifukwa sinizakupasani malo yake kunkala chintu chanu, chifukwa napasa Ar kuli bamubadwe wa Loti, kunkala chitntu chao.' >>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 <<<<<< HEAD ¹⁰ (Ma Emite banankala kuja kale, banthu wonveka, monga bambili, ndipo batali monga ma Anakim; ¹¹ aba nawo ni bozibika kuti niba Rephaim, monga ma Anakim; koma ma Moanite baitana beve kuti ma Emite. ===== ¹⁰ (Ba Emite banali kunkala kuja kudala, monga bantu bakulu, bambili, ndipo batali monga ba Anakimu; ¹¹ aba nabeve bali monga ba Rapaimu, monga ba Anakimu; koma baku Moabu baitaneni ba Emite. >>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 <<<<<< HEAD ¹² Ma Horite nawo banankala mu Seir kale, koma bana ba Esau bana pambana beve. Banabaononga beve kuchoka pasogolo pawo na kunkala mu malo mwawo, monga Israeli anachita ku malo yawo nakunkala noyo yamene Yehova anapasa kuli beve.) ===== ¹² Ba horite nabeve banali kunkala ku Seiri kudala, koma bamubadwe wa Esau bana pyanika beve. Bana baononga kuyambila banaliko beve bakalibe naku nkala mu malo yao, monga Israeli anachitila ku malo ya chitntu chamene Yehova anapasa kuli beve.) >>>>>> 31f2266056f1a583193e6f4b2d0ffec4c1748c84 ¹³ Manje nyamuka na kuyenda mumana wamanzi ku Zeredi.' ¹⁴ Ndipo tinayenda pamwamba pa Zeredi pochoka manzi. Manje masiku kuchoka pamene tinabwela kuchoka ku Kadeshi Barnea mpaka kuoloka ku mumana wamanzi wa Zeredi, zinali zaka seti-eiti. Inali pali ija ntawi kuti yonse mibadwo ya bamuna bali woyenela kumenya nkondo banayenda kuchoka ku banthu, monga Yehova analumbila kuli beve. ¹⁵ Koma, kwanja kwa Yehova kunali kosusana na uja mubadwe kuti abawononge kuchoka ku banthu mpaka bakanayenda. ¹⁶ Ndipo chinachitika, pamene bonse bamuna bali oyenela kumenyana banafa na kuyenda kuchoka pakati pa bathu, ¹⁷ kuti Yehova anakamba kuli ine, nakuti, ¹⁸ Imwe lelo mufunika kupita ku Ar, ku malile ya Moabu. ¹⁹ Mukabwela pafupi molanganana na banthu ba Ammon, musabavute beve kapena kumenyana nawo; chifukwa sinizapa imwe yaliyonse malo ba bathu ba Ammoni kunkala nayo; chifukwa naipasa ku bana ba Loti monga kunkala yawo. ²⁰ (Yaja futi yabelengewa kunkala malo yaba Refaimu. Ba Refaimu banali kunkala kuja kudala-koma ba Amori bama baitana zamuzummimu- ²¹ bantu monga bakulu, bambili, na batali monga Anakimu. Koma Yehova anaba ononga kukalibe ba Ammori, ndipo bana bapyanika nakunkala mu malo yao. ²² Ichi Yehova anachi chita nakuli bantu ba Esau, banali kunkala ku Seiri, pamene ana ononga ba Horite pamene kukalibe beve, na bamubadwe wa Esau banatenga malo kuli beve nakunkala mumalo ya mpaka lelo. ²³ Monga kuli ba Avvite banali kunkala mu minzi mpaka kufika ku Gaza, ba kapitorimu, banachokela ku kapito, bana ba ononga nakunkala mu malo yao.) ²⁴ ""

Manje nyamukani, yambamponi na ulendo wanu, nakupita ku chikwa cha baku Anoni; onani, napasa mumanja yanu Sihoni waku Amori, mfumu yaba Heshiboni, na malo yake. Yambani kuyatenga, nakumenyana naye mu nkondo. ²⁵ Lelo nizayamba kuika manta na kuyopa imwe pa bantu bali pansi pa myamba; bazanvela nkani pali imwe na njenjema nakunkala na manta kamba ka imwe.' ²⁶ Ninatuma bopeleka mau kuchokela mu chipululu cha Kademoti mapaka ku Sihoni, mfumu ya Heshiboni, na mau yamutendele, kukamba, ²⁷ 'lekani nipiteko mu malo yanu; nizapita naku nkala chabe pa panjila; sinizapindamukila ku kwanja ya manja olo yamanzele. ²⁸ Muzanigulisako vakudya pa ndalama, kuti ningadye; munipaseko manzi pa ndalama, kuti ningamwe; nilekeni chabe nipiteko na mendo; ²⁹ munga bamubadwe wa Esau banali kunkala ku Seiri, na baku Moabu banali kunkala ku Ar, banachitila kuli ine; mpaka ninapita ku Yodano mpaka mumalo yamene Yehova mulungu watu atipasa ife.' ³⁰ Koma Sihoni, mfumu ya Heshboni, sanafune kuleka ife kupitila kuli eve; chifukwa Yehova Mulungu wanu anayumisa maganizo yake na kulimbisa mutima wake, kuti iye angamugonjese mwa mpavu zanu, munga mwamene akuchita lelo. ³¹ Yehova anakamba kuli ine, 'Ona, Ine nayamba kupulumusa Sihoni na malo yake basogolo panu; yambani kutenga, kuti imwe mutenge malo yake.' ³² Mwaicho Sihoni anachoka mokangana naife, eve na bonse bantu bake, kumenyana pa Jahazi. ³³ Yehova mulungu watu anamupasa kuli ife ndipo tinamugonjesa na bana bake bamuna na bantu bake bonse. ³⁴ Tina tenga yonse mizinda yake pa ntau ija naku onongelatu mizinda yonse- bamuna na bakazi na bana bang'ono; sitinasiyeko opulumuka aliyense. ³⁵ Koma chabe vibeto tinatenga vapindu kuli ife, pamozi na va pindu vamu mizinda zamene tinatenga. ³⁶ Kuchoka ku Aroer, yamene ili mumbali mwa chigwa cha Arnon, na kuchoka ku munzi wamene uli muchigwa, kufikila ku Gileadi, kuja kunalibe munzi utali kwa ife. Yehova Mulungu wathu anatipasa mumanja mwathu. ³⁷ Kunali chabe ku malo ya wobadwa kwa Ammoni kwamene simunayende, munga kuli yonse mbali ya mumana wa Jabbok, na minzi ya ziko yapapili-Kulikonse Yehova Mulungu wathu analeta kuti tiyendemo.

Chapter 3

¹ Ndipo tinapindamuka na keyenda munjila yaku Bashani. Og, mfumu ya Bashani, anabwela na kuukila ife, iye na bonse bathu bake, kumenyana ku Edrei. ² Yehova anati kuli ine, 'Usamuyope; chifukwa napasa iwe kupambana pali eve ndipo naika bonse bathu bake na malo yake pansi paulamulilo wako. Uzachita kuli eve munga mwamene unachitila kuli Sihoni, mfumu yaku Amori, wamene anankala ku Heshbon.' ³ Ndipo Yehova Mulungu wathu anatipasa ife kupambana pali Og mfumu yaku Bashani, na bonse banthu bake banaikidwa pansi paulamulilo wathu. Tinabamenya mpaka kunalibe umozi wa banthu bawo anasala. ⁴ Tinatenga yonse minzi pali ija ntawi. Kunalibe kapena umozi pa minzi ili sikisite yamene sitinatenge kuchoka kuli beve-yonse malo ya Argob, mfumu yaku Og mu Bashani. ⁵ Izi zonse zinali mizinda zolimba navipupa vitali, makomo, na nsimbi; izi zinali kuchoselako yambili minzi yosachingilizwa na vipupa yamene tinatenga. ⁶ Tinaba onongelatu, munga tinachitila kuli Sihoni mfumu yaku Heshiboni, kuonongelatu muzinda uli onse- bamuna naba kazi na bana bang'ono. ⁷ Koma vibeto vonse na vintu va pindu vamu mizinda tanatenga kunkala vatu. ⁸ Pa ntau ija tinatenga malo kuchoka mu manja ya mfumu zibili za baku Amori, banali kusidya kwa Yodano, kuchokela ku chikwa cha Arnoni mpaka ku pili ya Hermoni ⁹ (pili ya Hemoni imaitaniwa kuti Sirioni nabaku Sidinia, na baku Amori bamaitana kuti Seiri) ¹⁰ na mizinda yonse yamu zigwa, Gileadi na Bashani, mpaka kufika ku Saleka na Ederei, mizinda ya ufumu wa Og ku Bashani." ¹¹ (Koma kwa osalila ba Rephaim, chabe Og mfumu ya Bashani ndiye anasala. Onani! Bedi yake inali bedi ya nsimbi. Nanga sikunali ku Rabbah, kwamene wobadwa kwa Ammoni bankala? Inali naini kubiti muutali na folo kubiti muufupi, mwamene banthu bamapimila.) ¹² " Aya malo tina tenga kunkala yatu pa ntau ija- kuchokela kuli Aroa, yamene yanali ku chikwa cha Amoni, na pang'ono ku ziko yakumapili ya Gileadi, na mizinda yake-ninapasa kuli bakuli Reubeni na kuli bakuli Gadi. ¹³ Bosala pali ba Gileadi na bonse ba Bashani, ufumu wa Og, ninapasa kujuba pakati mutundu wa Manasse. (Yonse malo ya Agobu, na Bashani. Malo ya mozi yaitaniwa malo ya Rafaimu. ¹⁴ Jairi, wa mubadwe wa Manasse, anatenga malo yonse ya Agobu kufikila naku malile ya baku Geshurite na Makatite. Anaitana malo, ngankale Bashani, muzina yake, Havvoti Jairi, mpaka lelo.) ¹⁵ Ninapasa Gilidi kuli Makir. ¹⁶ Kuli ba Rubenaiti na kuli ba Gadite ninapasa malo kuchoka ku chigwa chaku Arnoni-pakati pa chigwa pali malile ya malo na - ku kumumana wa Jabbok, yamene ndiye malile na wobadwa kuli Ammoni. ¹⁷ Inangu ya boda ilinso malo ya mumana wa Yodani, kuchoka ku Kinnereth kupita ku nyanja ya Araba (ija ndiye, nyanja ya muchele) mukutentemuka kwa pili ya Pisgah kumumawa. ¹⁸ Ninakuuzani pali ija ntawi, nakuti, 'Yehova Mulungu wanu akupasani aya malo kunkala yanu; imwe, bonse bamuna ba nkondo, bazapita wokonzeka pasogolo pa babale banu, banthu ba Israeli. ¹⁹ Koma bakazi banu, bana banu, na vibeto vanu (niziba kuti muli na vibeto vambili), viznkala mumizinda yanu yamene nakupasani, ²⁰ mpaka Yehova apase kupumula ku ba bale banu, munga achitila kuli imwe, mpaka nabeve batenge malo yamene Yehova mulungu wanu abapasa kuseli kwa Yodano; mwaicho muzbwelela, mwamuna aliyense pali imwe, kuvintu vanu vamene nakupasani.' ²¹ Ninauza Yoswa pali ija ntawi, nakuti, 'Yako menso yaona vonse vamene Yehova Mulungu wako achita kuli aya yabili mafumu; Yehova azachita chimozi mozi kuli yonse maufumu kwamene iwe uzayenda. ²² Iwe siuzayopa beve, chifukwa Yehova Mulungu wako niwamene azakumenyela iwe.' ²³ Ninamufunsa Yehova pali ija ntawi, nakuti, ²⁴ 'Imwe Ambuye Yehova, mwayamba kulangiza wanu wanchito ukulu wanu na kwanja kwanu kolimba; kodi nindani mulungu aliko kuja kumwamba kapena mu ziko lapansi wamene angachite ncito zimozi munga zamene mwachita, na machitidwe yampanvu ? ²⁵ Lekani ine niyende kuja, nakupapatani, na kuona malo yabwino yamene yapitilila ku Yodani, ija ziko yabwino yapapili, na futi Lebanoni.' ²⁶ Koma Yehova anali wokalisa na ine chifukwa cha imwe; Iye sananvele kuli ine. Yehova anakamba kuli ine, 'Leka ichi chinkale chokwana kwa iwe-usakambe nafuti vinangu kuli ine pali iyi nkani: ²⁷ Yenda pamwamba pa Pisgah na kunyamula menso yako kumazulo, kumumwela, kumupoto, na kumumawa; langana na menso yako, chifukwa iwe siuzayenda kuja ku Yodani. ²⁸ Koma, Langiza Yoswa na kumulimbisa, chifukwa azayenda basogolo pali aba bathu, ndipo azalengesa beve kuti batenge malo yamene uzaona.' ²⁹ Ndipo tinankala mu chigwa kulanganana na Beth Peor.

Chapter 4

¹ Manje, Israeli, nvelani ku malamulo yamene nifuna kukupunzisani, kuyachita; kuti munkale naumoyo na kuyenda na kunkala nayo malo yamene Yehova, Mulungu wa batate banu, akupasani imwe. ² Simuzaonjezelapo ku mau yamene nakuuzani, kapena imwe simuzachosapo, kuti musunge malamulo ya Yehovah Mulungu wanu yamene nili kufuna kukuuzani imwe. ³ Menso yanu yana ona vamene Yehova anachita chifukwa cha Baala Peori; kuli bonse bamuna banakonka Baala waku Peori, Yehova mulungu wanu aba ononga pakati pa imwe. ⁴ Koma imwe bana gwililila kuli Yehova mulungu wanu muli ba moyo lelo, aliyense pali imwe. ⁵ Onani, nakupunzisani malamulo na vokonka, monga mwamene Yehova mulungu wanga ananilamulila ine, kuti mungachite ichi pakati pa malo yamene mungenamo nakuyatenga. ⁶ Mwaicho yasungeni naku yachita; chifukwa ichi ndiye nzelu zanu na chinveseso chanu pamenso pa bantu bamene baza nvela pali ivi vonse va malamulo vamene nakamba, 'Zoona iyi ni ziko ya mpanvu na nzelu na bantu bachinveseso.' ⁷ Chifukwa ni iti ziko yampanvu yamene ili naka mulungu kali pa fupi na beve, monga Yehova mulungu watu alili ntau iliyonse tika muitana eve? ⁸ Ndi yiti ya mpanvu iliko yamene ili nama lamulo na vokonka vo yela monga yonse aya malamulo yamene ni ika pasogolo panu imwe lelo? ⁹ Ikilani chabe nzelu nakuzisunga mweka, kuti musaibale vintu vamene menso yanu yana ona, kuti visachoke mumitima mwanu kwa masiku yonse ya umoyo wanu. Mwaicho, lekani vizibike kubana banu naku bana ba bana banu. ¹⁰ Pasiku yamene muna imilila pasogolo pa Yehova mulungu wanu ku Horebu, pamene Yehova anakamba kuli ine, 'Ni unjikile bantu, nizabapanga kuti ba nvele mau yanga, kuti bapunzile kuniyopa masiku yonse yamene bali na moyo pa ziko yapansi, nakuti bangapunzise bana bao.' ¹¹ Munabwela pafupi naku imilila munyansi mwa lupili. Lupili inali kupya na mulilo mpaka kumwamba, na mudima, kumbi, na mudima ukulu. ¹² Yehova anakamba kuli imwe kuchokela pakati pa mulilo; muna nvela liu na mau yake, koma simuna one chili chonse; muna nvela chabe liu. ¹³ Anakamba kuli imwe chipangano chake chamene anakuuzani kuti muchite, malamulo yali teni. Anayalemba pa bili pa mwala. ¹⁴ Yehova analamulila ine pali ija ntawi ku punzisa imwe zoikika na malamulo, kuti imwe muyachite mu malo yamene mupitamo na kuyatenga. ¹⁵ Ndipo tengani kunvesesa kukulu kwaimwe mweka-chifukwa munaona kulibe kanthu pasiku yamene Yehova anakamba kuli imwe pa Horebu kuchoka mukati mwa mulilo- ¹⁶ kuti musaziononge mweka na kupanga chosema chifanizilo chooneka monga chintu, chofafaniza monga mwamuna kapena mukazi, ¹⁷ chifanizilo cha iliyonse nyama ili paziko yapansi, chifanizilo cha iliyonse yamapepe nyoni yamene imbululuka mu mwamba, ¹⁸ chifanizilo cha chilichonse chamene chikalaba pa doti, kapena chifanizilo cha iliyonse nsomba yamene ili mu manzi pansi pa ziko yapansi. ¹⁹ Simuzanyamula menso yanu ku mwamba na kulangana pa zuba, pa mwezi, kapena pa nyenyezi-yonse magulu yaku mwamba—na kufendeza kutali ku lambila ivo na kuvilemekeza—Ivo vinthu vamene Yehova Mulungu wanu akupasani monga gawo kuli bonse banthu bali pansi pa kumwamba. ²⁰ Koma Yehova atenga imwe na kukutulusani imwe ku nsimbi yakupya, kuchoka ku Igupto, kunkala kuli eve banthu bali bake, monga mulili lelo. ²¹ Yehova anali wokalipa na ine chifukwa cha imwe; analumbila kuti nisayende kuja ku Yodani, na kuti nisayende mu malo yabwino, malo yamene Yehova Mulungu wanu akupasani imwe monga yanu. ²² Koma, nifunika kufela muno mumalo; sinifunika kuyenda kuja ku Yodani; koma imwe muzayenda kuja na kutenga yaja malo yabwino. ²³ Ikilani nzelu kuli imwe mweka, kuti musa ibale chipangano cha Yehova mulungu wanu, chamene anapanga na imwe, nakuzipangila mweka chaoneka cho beza kupalanisa chili chonse chamene Yehova anakulesani kupanga. ²⁴ Chifukwa Yehona nimulilo onyekesa, ni mulungu wa kaduka. ²⁵ Ngati mwankala na bana naba zukulu, ngati mwankala mu malo ntau itali, ndipo mwalakwisa mweka nakupanga chobeza kupalanisa na chili chonse, nakuchita choipa pamenso pa Yehova mulungu wanu, kumuyamba kuti akwiye- ²⁶ Ni itana mwamba na ziko yapansi kunkala mboni chifukwa cha imwe lelo kuti manje manje mukakamba mu onongeke kuchoka mu malo yamene muyendamo kutenga kupitilila Yodano; simuzapakisa masiku yanu muja, koma muza onongekelatu. ²⁷ Yehova azakumwazani imwe mukati mwa banthu, ndipo muzasala ban'gono mu namba mu maziko, kwamene Yehova azakusogolelani kutali. ²⁸ Kuja muzatumikila mulungu inagu, nchito za bamuna zamanja, nkuni na myala, vamene siviona, kunva, kapena kunusha. ²⁹ Koma kuchoka kuja muzasakila Yehova Mulungu wanu, ndipo muzamupeza, ndipo mukamufuna pambuyo pake na mutima wanu wonse na bonse moyo wanu. ³⁰ Koma mukankala mu mavuto, ndipo kapena vonse ivi vinthu vifuna vabwela pali imwe, muli ayo masiku yosiliza muzabwelela kuli Yehova Mulungu wanu na kunvela ku mau yake. ³¹ Chifukwa Yehova Mulungu wanu ni Mulungu wachifundo; Sazakulepelani imwe kapena kukuonongani, kapena kuibala chipangano cha batate banu chamene analumbila kuli beve. ³² Funsani manje pa zamasiku yamene yanapita, yamene yanali pasogolo pa ntawi yanu, kuchokela pa siku yamene Mulungu anapanga munthu pa ziko lapansi, funsani kuchoka kumoji kosilila kumwamba kufikila na kwingu, kapena kunali chilichonse chamene chinali chikulu monga ichi, kapena kuli chilichonse monga ichi chinanvekapo? ³³ Ushe kuli banthu bananvela mau ya Mulungu akamba

kuchokela mukati mwa mulilo, monga imwe mwanvelela, na kunkala? ³⁴ Kapena kuti Mulungu anachiyesapo kuyenda na kutenga kwa iye yeka ziko kuchoka mukati mwa inangu ziko, mwa mayeso, mwa visanzo, na mwa zodabwisa, na mwa nkondo, na mwa kwanja kwampavu, na motambasula kwanja, na mwa zoyofya zikulu, monga zilizonse zamene Yehova Mulungu wanu anachita kwa imwe mu Igupto pa menso yanu? ³⁵ Kuli imwe ivi vintu vina onekela, kuti muzibe kuti Yehova ni mulungu, nakuti kulibe wina kunja kwa eve. ³⁶ Kuchokela kumwamba analengesa kuti munvele liu yake, kuti anga ku uzeni vochita; pa ziko analengesa kuti mu one mulilo wake; muna nvela mau yake kuchokela pakati pa mulilo. ³⁷ Chifukwa anakonda ba tate banu, anasanka mubadwe unakonka beve, naku kuchosana mu Iguputo mukupezekapo kwake, na mpanvu zake zikulu, ³⁸ kuti achose pasogolo panu maziko yakulu na mpanvu kuchila imwe, kuku letani mukati, ku kupasani malo yao kunkala chopyanika, mpaka lelo. ³⁹ Zibani kuchokela lelo, nakuika muitima yanu, kuti Yehova ni mulungu kumwamba na pansu pa chalo; kulibe wina. ⁴⁰ Muza sunga vokonka na malamulo yake yamene nikulamulani lelo, kuti vinga yende bwino kuli imwe na ku bana banu kusogolo kwanu, kuti munga pakise masiku yanu mu malo yamene Yehova mulungu wanu akupasani imwe kwamu yayaya." ⁴¹ Ndipo Mose anasanka itatu minzi kumbali yaku mumawa ya Yodani, ⁴² kuti aliyense afunika kutamangila ku munzi umozi wa minzi ngati apaya winangu mosaziba, kopanda kunkala mudani wake kumbuyo. Mu kutamangila ku umozi mwa iyi minzi, angapulumuke. ⁴³ Inali: Beze mu chipululu, ziko ya chigwa, yaba Rubenaiti; Ramoth mu Gilidi, kwaba Gadite; na Golani mu Bashani, kwaba Manassites. ⁴⁴ Iyi ndiye lamulo yamene Mose anaika pasogolo pa banthu ba Israeli; ⁴⁵ Aya ndiyo malemba yachipangano, malamulo, na yonse malemba yamene anakamba ku banthu ba Israeli pamene banachoka ku Igupto, ⁴⁶ pamene banali ku mumawa kwa Yodani, mu chigwa cholanganana na Beth Peor, mu malo ya Sihon, mfumu ya Amori, wamene anankala ku Heshbon, wamene Mose na banthu ba Israeli bagonjesa pamene banachoka ku Igupto. ⁴⁷ Bana tenga malo yake kunkala yao, na malo ya Og mfumu ya Beshani- izi, mfumu zibili za baku Amori, banali kujumpa Yodano chaku maba. ⁴⁸ Iyi ziko inali kuchokela ku Aroer, kumbali kwa chikwa cha Armoni, mpaka ku mpili ya Siyoni(olo pili ya Hermoni), ⁴⁹ naku ikilapo vigwa vonse va mumana wa chikwa cha Yodano, kumaba kuseli kwa Yodano, ku nyanja ya Araba, mpaka ku mushelemuko wa Pisiga.

Chapter 5

¹ Mose anaitana ba Israeli bonse nakukamba kuli beve, " Nvelani, Israeli, kuvo funika kukonka na malamulo yamene niza kamba mu matu mwanu lelo, kuti mungaya punzile na kuyasunga. ² Yehova mulungu watuanapanga chipangano naife ku Horebu. ³ Yehova sanapange chipangano namakolo yatu, koma naife, bonse tili na moyo lelo. ⁴ Yehova anakamba naimwe menso na menso pa lupili kuchoka mukati mwa mulilo ⁵ (Ninaimilila pakati pa Yehova na imwe pali ija ntawi, kuvumbulusa kuli imwe mau yake; chifukwa munali na manta chifukwa cha mulilo, ndipo simunayende pamwamba pa lupili). Yehova anati, ⁶ 'Ndine Yehova Mulungu wanu, wamene anakuchosani ku ziko ya Igupto, kuchoka mu nyumba ya ukapolo. ⁷ Simuzankala na milungu inangu pasogolo panga. ⁸ Imwe simuzapanga kwa imwe mweka chosema chooneka kapena chilichonse chofanizila cha chilichonse chamene chili kumwamba, kapena chamene chili mu ziko lapansi, kapena chamene chili pansi pa manzi. ⁹ Simuzagwada pansi kuli beve kapena kusebenzela beve, chifukwa ine, Yehova Mulungu wanu, ndine Mulungu wa jelasi. Nimapasa chilango pa kuchimwa kwa makolo paku leta chilango pa bana, kufikila wachitatu na wanamba folo mubadwe kuli awo bamene bazonda ine, ¹⁰ na kulangiza chamuyaya chikondi kuma sauzande, kuli awo bamene bakonda ine na kusunga malamulo yanga. ¹¹ Imwe musatenge zina ya Yehova Mulungu wanu mwa chabe, chifukwa Yehova sazaleka kumugwila mulandu wamene atenga zina yake mwachabe. ¹² Sungani siku ya Sabata kuisunga inkale yoyela, monga Yehova Mulungu wanu alamulila imwe. ¹³ Pa masiku yali sikisi muzasebenza na kugwila zonse nchito zanu; ¹⁴ koma siku ya namba seveni ni sabata kwa Yehova Mulungu wanu. Pali iyo simufunika kuchita iliyonse nchito- osati imwe, kapena bana banu bamuna, kapena bana banu bakazi, kapena banchito banu bamuna, kapena banchito banu bakazi, kapena ng'ombe zanu, kapena mabulu yanu, kapena iliyonse nyama yanu, kapena mulendo wamene ali mukati mwa geti yanu. Ichi nichakuti banchito banu bamuna na bakazi banchito bangapumule monga na imwe. ¹⁵ Muzaitanila kunzelu kuti munali ba kapolo mu ziko ya Igupto, ndipo Yehova Mulungu wanu anakuchosani imwe kuchoka kuja na kwanja yampanvu na kotambuluka kwanja. Ndiponso Yehova Mulungu wanu alamulila imwe kusunga siku ya sabata. ¹⁶ Lemekezani batate banu na bamai banu, monga Yehova Mulungu wanu alamulila imwe kuchita, kuti munkale ntawi yaitali mu ziko yamene Yehova Mulungu wanu akupasani, na kuti viziyenda bwino naimwe. ¹⁷ Iwe siuzapaya. ¹⁸ Siuzachita chigololo. ¹⁹ Siuzaba. ²⁰ Siuzapasa umboni waboza mosusana na wapafupi panu. ²¹ Iwe siuzatengela mukazi wa munzako, siuzapasula nyumba ya munzako, munda wake, kapena wanchito bake bamuna, kapena wanchito wake mukazi, ng'ombe zake, kapena ma bulu yake, kapena chilichonse chamene chili chamunzako. ²² Aya mau Yehova anayakamba monveka kuli bonse banasonkana palupili kuchoka pakati pa mulilo, yamu makumbi, na chimudima chikulu; sanafakilepo yaliyonse yambili mau. Analemba ayo pansi pa mwala na kubapasa beve. ²³ Kunabwela kuti, pamene munanvela mau kuchokela mukati mwa mudima, pamene lupili lunali kupya, kuti munabwela pafupi naine- bonse bakulu banu na wosogolela ba mitundu yanu. ²⁴ Munakamba kuti, 'Onani, Yehova Mulungu wathu atilangiza ife ulemelelo wake na ukulu wake, ndipo tanvela mau yake kuchoka mukati mwa mulilo; taona lelo kuti Mulungu amakamba na bathu, bangankale namoyo. ²⁵ Nanga nichani chamene tingafele? Chifukwa uyu mulilo ukulu uzatishoka ife; ngati tanvela mau ya Yehova Mulungu wathu mopitilila, tizamwalila. ²⁶ Nanga nindani kumbali kwatu aliko pakati pa yonse tupi wamene ananvela mau ya Mulungu wamoyo akamba kuchoka mukati mwa mulilo na kunkala naumoyo, monga mwamene tachitila? ²⁷ Monga kuli imwe, mufunika kuyenda na kunvela kuli vilivonse vamene Yehova Mulungu wanu akamba; mubwezepo kwa ife vilivonse vamene Yehova Mulungu wanu akamba kuli imwe; tizanvela kuli icho na kukonka. ²⁸ Yehova ananvela mau yanu pamene munakamba kuli ine. Anakamba kuli ine, Nanvela mau ya aba bathu, vamene banakamba kuli iwe. Vamene banakamba vinali bwino. ²⁹ Ya, kapena kunali monga wachonco mutima muli beve, kuti banganilemekeze ine na lyonse kusunga malamulo yanga, kuti zizibayendela bwino na bana bawo muyayaya! ³⁰ Yenda nakuuza beve, "Bwelelani ku misasa yanu." ³¹ Koma kuli imwe, imililani pano naine, ndipo nizakuuzani yanse malamulo, zoikika, na zokambidwa zamene muzabapunzisa beve, kuti bayasunsunge ayo mu malo yamene nizabapasa kuti batenge. ³² Muzasunga, chamene Yehova Mulungu wanu akuuzani; Simuzapindamukila kumbali inangu ku kwanja lamanja kapena kukwanja lamanzele. ³³ Muzayenda muli zonse njila zamene Yehova Mulungu wanu akuuzani, kuti munkale namoyo, ndipo kuti ziyende bwino naimwe, nakuti yayende pasogolo masiku yanu mu malo yamene muzatenga.

Chapter 6

¹ Manje aya ndiyo malamulo, malangizo, na malemba yamene Yehova Mulungu wanu auza ine kuti nikupunziseni, kuti imwe musunge mu malo yamene muyendamo kuja ku Yodani mukutenga; ² Kuti imwe mutokoze Yehova Mulungu wanu, na kuti musunge vonse malangizo na malamulo yamene nikuuzani - imwe, bana banu bamuna, na bana banu bamuna bana bawo bamuna, yonse masiku ya umoyo wanu, kuti masiku yanu yapitilile. ³ Mwaichi nvelani kuli beve, Israeli, na kuyasunga, kuti zingayende bwino naimwe, nakuti munganveke nakuchuluka, mu malo yochosa mukaka ndi uchi, monga Yehovah, Mulungu wa batate banu, alonjeza kuti muzachita. ⁴ Nvelani, Israeli: Yehova Mulungu wathu ali umozi. ⁵ Muzakonda Yehova Mulungu wanu na mutima wanu wonse, na umoyo wanu wonse, na zonse mpavu zanu. ⁶ Mau yamene nikuuzanu imwe lelo yazankala mu mitima yanu; ⁷ ndipo mwachangu muzayapunzisa kuli bana banu; muzakamba pali yeve pamene munkala munyumba mwanu, pamene muyenda mumuseu, pamene mugona, na pamene munyamuka. ⁸ Muzayamanga yeve monga chowonesela pa manja yanu, ndipo chizatumikila monga chapasogolo pakati pa menso yanu. ⁹ Muzayalemba pa viseko vanu va panyumba zanu na pama geti yanu. ¹⁰ Ngati Yehova Mulungu wanu akubwelesani mu malo yamene analumbila kuli batate banu, kuli Abrahamu, kuli Isaki, na kuli Yakobo, kuti azakupasani, na yikulu na yabwino minzi yamene simunamange, ¹¹ na manyumba yozula na vonse vosiyana siyana vabwino vintuvamene simunapange, visime vamanzi vamene simunakumbe, na minda na mitengo za olivu zamene simunashange, muzadya ndiponso muzakuta- ¹² koma munkale ochenjela kuti musaibale Yehova, wamene anakuchosani imwe ku ziko ya Igupto, kuchoka ku nyumba ya ukapolo. ¹³ Muzalemekeza Yehova Mulungu wanu; iye muzamutokoza, ndipo muzalumbila pa zina yake. ¹⁴ Simuzayenda pambuyo pa inangu milungu, milungu ya bathu bamene bonse wokuzungulilani-- ¹⁵ chifukwa Yehova mulungu wanu wamene ali pakati panu ni Mulungu wa jelasi-- ngati mwachita, ukali wa Yehova Mulungu wanu uzaukila mosusana na imwe ndipo azakuonongani imwe kuchoka pa ziko yapansi. ¹⁶ Simuzamuyesa Yehova Mulungu wanu monga mwamene munamuyesela ku Massah. ¹⁷ muzafunika mwachangu kusunga malamulo ya Yehova Mulungu wanu, yachifundo malamulo, na malangizo, yamene akulamulilani imwe. ¹⁸ Muzachita zamene zili zolungama ndiponso zabwino pa menso ya Yehova, kuti zizikuyendelani bwino imwe, ndipo kuti muyende mukati na kutenga malo yamene Yehova analumbila kuli batate banu, ¹⁹ kuchosa bonse badani banu kuchoka pasogolo panu, monga Yehova akambila. ²⁰ Koma mwana wako mwamuna akafunsa mu ntawi yobwela, nakuti, 'Kodi nichipangano bwanji chokambidwa, choikika, na vinangu vokambidwa vamene Yehova Mulungu wathu akulamulilani imwe?' ²¹ Ndipo uzakamba kwa mwana wako mwamuna, 'Tinali bakapolo ba Farao mu Igupto; Yehova anatichosa ife kuchoka mu Igupto na kwanja kwa mpavu, ²² ndiponso analangiza zooneka na zodabwisa, vikulu ndiponso voyofya, pali Igupto, pali Farao, na pali bonse bamu nyumba yake, pasogolo pa menso yathu; ²³ na kutichosa ife kuchoka kuja, kuti atibwelese ife mukati, kutipasa ife malo yamene analumbila kuli batate bathu. ²⁴ Yehova anatilamulila ife kuti ntawi zonse tisunge yonse malamulo, kuyopa Yehova Mulungu wathu nichabwino kwaife, ndiye kuti atisunge ife naumoyo, monga mwamene tilili lelo. ²⁵ ngati tasungu yonse aya malamulo basogolo pa Yehova Mulungu wathu, monga mwanene atilamulila ife, ichi chizankala kuyela kwathu.'

Chapter 7

¹ Pamene Yehova Mulungu wanu akubwelesani mu malo kuti muyende nakunkala nayo, azachosa yambwili ma ziko pasogolo panu- ma Hittites, ma Girgashites, ma Amori, ma Kananaiti, ma perizziti, ma Hivaiti, na ma Jebusaiti- seveni maziko yonveka ndiponso yamphavu kuchila imwe. ² Ni Yehova Mulungu wanu wamene azapasa beve kwa iwe pamene mukagonjesa beve, ndipo mufunika kusilizilatu kubaononga beve. Simuzapanga chilichonse chipangano na beve, na kubalangiza beve chifundo. ³ Kapena imwe kusunikaniza vikwati na beve. Simuzapasa bana banu bakazi kuli bana bawo bamuna, na imwe simuzatenga bana bawo bakazi kwa bana banu bamuna. ⁴ Chifukwa sibazapindamukisa kwinangu bana banu bamuna kuchoka mukukonka ine, kuti bakalambile inangu milungu. chifukwa ukali wa Yehova uzanyamukila mukususana nabeve, ndipo azaononga imwe mwamusanga. ⁵ Ivi ndiye vamene muzabachita beve: Muzaononga maguwa yawo, kupwanya myala yoimilila yawo mutung'ono, kujuba pansi vawo voimilika Ashera, na kushoka yawo milungu. ⁶ Chifukwa ndimwe ziko yamene ili yopatulika kwa Yehova Mulungu wanu. Akusankani imwe kunkala banthu kwa Iye kutenga, kuchila bonse benangu bathu bamene bali paziko yapansi. ⁷ Yehova sanaike chikondi chake pali imwe kapena kusanka imwe chifukwa munali bambili mu mabelengedwe kuchila benangu banthu--- koma ndimwe munali bang'ono pali banthu bonse- ⁸ koma chifukwa akukondani, ndipo anaganiza kuti asunge kulumbila kwamene analumbila kuli batate banu. Ichi ndiye chifukwa chake Yehova akuchosani imwe na kwakwanja kwampantu na kukupulumusani imwe kuchoka ku nyumba ya ukapolo, kuchoka ku manja ya Farao, mfumu ya Igputo. ⁹ Mwaichi zibani kuti Yehova Mulungu wanu- ni Mulungu, Mulungu wokulupilika, wamene asunga chipangano ndiponso wokulupilika kwa mibadwe ma sauzande kuli awo bamene bamukonda na kusunga malamulo yake, ¹⁰ koma abwezela bamene bamuzonda pamenso pabo, kubaononga beve; sazankala nachifundo kuli aliyense wamene amuzonda iye; azamubwezela eve pamenso pake. ¹¹ Mufunika mwaichi kusunga malamulo, zoikika, na zokambidwa zamene nikulamulilani imwe lelo, kuti imwe musavichite. ¹² Ngati mwanvela kuli izi zokambidwa, na kusunga na kuzichita izo, chizachitika kuti Yehova Mulungu wanu azasunga na imwe chipangano na kukulupilika kwake kwamene analumbila kuli batate banu. ¹³ Azakukondani, azakudalisani, na kukuchulukisani imwe. Azadalisa zipaso za mumimba yanu, zipaso za muntaka yanu-- tiligu yanu, waini yasopano, na mafuta yanu- mosungila ng'ombe zanu na zing'ono mu malo yamene analumbila kuli batate banu kupasa imwe. ¹⁴ Muzadalisika kuchila bonse benangu banthu; Sikuzankala wamene azankala mwamuna alibe mwana kapena wosabala mukazi pakati pa imwe kapena pa zobeta zanu. ¹⁵ Yehova azachosapo pali imwe matenda; palibe pali yoipa matenda yaku Igputo yamene mwaziba yazaikidwa pali imwe, koma azayaika pali awo bonse bamene bazonda imwe. ¹⁶ Muzaononga bonse bathu bamene Yehova Mulungu wanu azapasa kwa imwe, ndipo menso yanu siyazanvela chifundo pali beve. Simuzalambila milungu yawo, chifukwa icho chizankala musampa kwa imwe. ¹⁷ Ngati wakamba mumutima wako, 'Aya maziko yambili yonveka kuchila ine; ningayachose bwanji? - ¹⁸ usayayope yameneayo; uzaitanila kunzeli chamene Yehova Mulungu wako anachita kuli Farao na kuli yonse Ijipito; ¹⁹ kusauka kukulu kwamene menso yako yanaona, zizindikilo, zodabwisa, kwanja kwampavu, na kotambuluka kwanja kwamene Yehova Mulungu wanu anachosela imwe. Yehova Mulungu wanu azachita chimozi kuli bonse bathu bamene muyopa. ²⁰ Mwaichi, Yehova Mulungu wanu azatuma mulimo pakati pawo, kufikila awo bonse wosala na bamene bazibisa beka kuchoka kuli imwe baonongeke kuchoka pamenso panu. ²¹ Simuzankala bamanta pali beve, chifukwa Yehova Mulungu wanu ali pakati panu, wa mukulu ndiponso woyopewa Mulungu. ²² Yehova Mulungu wanu azachosa panja yonse maziko basogolo panu pang'ono pang'ono. Simuzabaononga awo bonse pantawi imozi, kapena nyama zamusanga zingabwele zambili kukuzungulilani imwe. ²³ Koma Yehova Mulungu wanu azakupasani imwe kugonjesa pali beve mukakumana nawo munkondo; azabasokoneza kwa kukulu mpaka bakaonongeke. ²⁴ Azaika mafumu yawo pansi pa mpavu zanu, ndipo muzapanga mazina yawo kuonongeka kuchoka paziko lapansi. Kuli olo umozi wamene azakwanisa kuimilila pasogolo panu, mpaka mukabaononga beve. ²⁵ Muzashoka vosema vawo va milungu yawo- musachinje siliva kapena golide yamene ibavininkila beve na kuitenga kunkala yanu, chifukwa mukachita ichi, muzankala ogwilidwa nachamene icho-- chifukwa nichosebanisa kwa Yehova Mulungu wanu. ²⁶ Simuzabwelesa chosebanisa munyumba na kuyamba kuchilambila. imwe muzaipisa na kuononga, chifukwa nichopatulidwa mu kuononga.

Chapter 8

¹ Mufunika kusunga yonse malamulo yamene nikupasani imwe lelo, ndiye kuti munkale na moyo na kuchuluka, na kuyenda mukati na kutenga malo yamene Yehova Mulungu analumbila kwa batate banu. ² Muzaitanila ku nzelu zonse njila zamene Yehova Mulungu wanu akusogolelani izi zaka zili fote muchipululu, kuti akupangeni munkale ozichepesa, kuti akuyeseni kuti azibe zamene zili mumutima wanu, ngati nizoona mungasunge malamulo kapena iyai. ³ Anakuchepesani, na kupangani imwe kunvela njala, na kukudyesani imwe ndi mana, yamene imwe simunazibe na yamene batate banu sibanaizibe. Anachita icho kuti akupangeni imwe kuziba kuti sibuledi yeka ingalengese munthu kunkala namoyo; koma, ni muli chilichonse chamene chichoka mukamwa ka Yehova kuti munthu angankale naumoyo. ⁴ vovala vanu sivinasile na kugwa kuchoka kuli imwe, na mendo yanu siyanavimbe muli izo zaka zili fote. ⁵ Muzaganiza pali ichi mumutima, bwanji, monga mwamuna apunzisa mwana wake, nayenso Yehova Mulungu apunzisa imwe. ⁶ Muzasunga malamulo ya Yehova Mulungu wanu, kuti muyende munjila zake na kumulemekeza iye. ⁷ Pakuti Yehova Mulungu wanu alikulowetsani m'dziko lokoma, dziko la mitsinje yamadzi, la akasupe, ndi akasupe oyenda m'zigwa ndi zitunda; ⁸ dziko la tirigu ndi barele, la mipesa, mkuyu, ndi makangaza; dziko la mitengo ya azitona ndi uchi. ⁹ Aya ni malo yamene simuzadya buledi mu njala ndipo simuzasoba kanthu kalikonse; malo yamene myala niyopangidwa ndi nsimbi, na kuchoka ma chulu yake mungakumbe mwala wa kopa. ¹⁰ Muzadya ndiponso muzakuta, ndipo muzadalisa Yehova Mulungu wanu pa yabwino malo yamene akupasani imwe. ¹¹ Munkale wosamala kuona kuti simunaibale Yehova Mulungu wanu, mu kulepela kusunga malamulo na zolamulila zake na zoikika zamene nikulamulilani imwe lelo. ¹² Chifukwa, mukadya ndiponso mwakuta, ndiponso mukamanga yabwino manyumba na kunkalamo, mitima yanu izanyamuka. ¹³ Nkalani wosamala pamene zobeta na ng'ombe zanu zikapaka ndiponso siliva na golide yanu ikachuluka, na vonse mulinavo vikachuluka, ¹⁴ ndipo mitima yanu inkala yonyamuka pamwamba na kuibala Yehova Mulungu wanu, wamene anakuchosani imwe ku ziko ya Igputo, kuchoka mu nyumba ya ukapolo. ¹⁵ Musamuibale iye wamene anakusogolelani imwe kupita mu chikulu ndipo choyofya chipululu, pamozi na zinkali njoka na sikopiyoni na malo yoyuma kwamene kunalibe manzi, wamene anakubweleselani manzi kuchoka mu mwala wokosa. ¹⁶ Anakudyesani imwe mu chipululu na mana yamene makolo banu sibanaizibe, kuti akuchepesani imwe na kukuyesani imwe, kukuchitilani imwe zabwino pakusiliza kwake, ¹⁷ koma mungakambe mumutima yanu, 'mpavu zanga na kwampanvu kwanja kwanga kwasebenzela konse uku kulemela.' ¹⁸ Koma muzaganiza mu nzelu Yehova Mulungu wanu, chifukwa niwamene wamene akupasani imwe mpavu zotenga chuma; kuti ankazikiseni chipangano chake chamene analumbila kuli batate banu, monga chilili lelo. ¹⁹ chizachitika ngati, ngati muzaibala Yehova Mulungu wanu na kuyenda pambuyo pa inangu milungu, kuipembeza, na kuilemekeza iyo, nizachita umboni mosusana na imwe lelo kuti zoona muzaonongeka. ²⁰ Monga ma ziko yamene Yehova ayapanga kuonongeka pasogolo panu, nanga imwe muzaonongka, chifukwa simunafune kunvela ku mau ya Yehova Mulungu wanu.

Chapter 9

¹ Nvelani, Israele; muli pan'gono nakujumpa Yolodani lelo, kuyenda mukati na kutenga ma ziko yakulu kuchila imwe ndiponso yamphavu kuchila imwe, na mizinda yamene ili yonveka ndipo yochingiliziwa kufika kumwamba, ² banthu wonveka ndiponso batali, bana bamuna ba Anakimu, wamene imwe muziba, ndipo uyo wamene munvela bantu kumukambapo, 'Nindani angaimilile pasogolo pa bana bamuna ba Anaki?' ³ Zibani mwaichi lelo kuti Yehova Mulungu wanu ndiye wamene ayenda pasogolo panu monga woononga mulilo; azabaononga iwo, nakugwesa beve pasogolo panu; ndipo muzabachosa beve panja na kubapanga beve kuonongeka mwamusanga, monga Yehova akambila kuli imwe. ⁴ Musakambe mumutima yanu, pambuyo Yehovah Mulungu wanu abawononga beve kubachosa kuchoka pasogolo panu, 'Chinali chifukwa cha kuyela kwanga chamene Yehova abwelesa ine kungwena muno na kutenga yano malo; ndiye chifukwa cha kuchimwa kwa aya ma ziko yamene Yehova ayachosa kuchoka pasogolo panu. ⁵ Sindicho chifukwa cha kulungama kwanu kapena kukoma mutima wanu kuti muyenda mukati na kutenga malo, koma chifukwa cha kusalungama kwa aya maziko yamene Mulungu wanu ayachosamo kuchoka basogolo panu, na kuti anga pange kubwela ya zoonu mau yamene analumbila kuli makolo yanu, kuli Abrahamu, Isake, na Yakobo. ⁶ Muzibe sopano, kuti Yehova Mulungu wanu sakupasani imwe aya malo kuti mutenge chifukwa cha chilungamo chanu, chifukwa ndimwe banthu wosanvela. ⁷ Kumbukilani ndipo musaibale mwane imwe munasokoneza Yehova Mulungu wanu kukalipa muchipulu; kuchokela pa siku yamene imwe munachoka mu ziko ya Igputo mpaka imwe mubwela kuli yano malo, imwe mwankala osanvela mukusana na Yehova. ⁸ Napaja pa Horebu imwe munakalipisa Yehova ku ukali, ndipo Yehova anakalipa kwambili na imwe kuti akuonongeni imwe. ⁹ Pamene ninayenda pamwamba pa lupili mukulandila malamulo pa mwala, malamumulo ya chipangano yamene Yehova anapanga kwa imwe, ninankala pa lupili kwa kwa masiku yali fote na usiku ili fote; sininadye ngankale buledi kapena kumwa manzi. ¹⁰ Yehova ananipasa ine zolembewa zibili za mwala zolembewa na chimbombo chake; pali ivo panalembewa vilivonse monga mwamene yonse mau yamene Yehova anaulusa kuli imwe pa lupili kuchoka mukati mwa mulilo pa siku yo sonkana. ¹¹ Chinachitika pakusila kwa masiku ayo yali fote na usiku uli fote kuti kuti Yehova ananipasa yabili volembelapo ya mwala, volembelapo ya chipangano. ¹² Yehova anakamba kuli ine, 'Nyamuka, yenda pansi mwamusanga kuchoka kuno, kubanhu bako, bamene munachosa ku Igputo, bazionongela beka. Bachita mwamusanga kupindamukila kumbali kuchoka munjila yamene ninalamulila iwo. Bazipangila beka chinthu.' ¹³ Mopililapo, Yehova anakamba naine na kuti, 'nabaona aba bathu; nibanhu bamene bali na ntonta. ¹⁴ Nisiye ine neka, kuti nibaononge beve na kuchosa zina yawo kuchoka pansi pa ziko yakumwamba, ndipo nizapanga iwe ziko yampavu ndipo yonveka kuchila beve.' ¹⁵ Ndipo ninapindamuka na kubwela pansi kulupili, ndipo lupili lunali kupya. Mapilisi yabili ya chipangano yanali mumanja yanga. ¹⁶ Ninalangana, ndipo onani, munachimwila mukususana na Jehova Mulungu wanu. Munazipangwila mweka mwana wa ng'ombe. Munapindamukila mwamusanga kumbali kuchoka mu njila yamene Yehova analamulila imwe. ¹⁷ Ninatenga mapilisi yabili na kuyataya kuchochoka mumanja mwanga. Ninayapwanya basogolo ba menso yanu. ¹⁸ Nafuti ninagona pansi pamenso pa Yehova masiku yali fote na usiku uli fote; sininadyepo ngankale buledi kapena kumwa manzi, chifukwa cha wonse uchimo wanu wamene munachita, mukuchita chija chamene chinali choipa pa menso ya Yehova, mwa kuti mumukalipise ku ukali. ¹⁹ Chifukwa ninali namanta ya ukali na kupya kosakondwela kwamene Yehova anali wokalipa kwambili mosusana naimwe kuti akuonongeni. Koma Yehova ananvela kwa ine ija ntawi futi. ²⁰ Yehova anali wokalipa kwambili na Aaroni nafuti pali yamene ija ntawi. ²¹ Ninatenga uchimo wanu, mwana wa ng'ombe wamene munapanga, na kumushoka, kukamenya, na kukagaya kang'ono, mpaka kanankala monga doti. Ninataya doti yake mu mumana wamene unachokela pansi kuchoka kulupili. ²² Ku Tabera, ku Massa, na ku Kibroth Hattaava, munakalipisa Yehova to mukwiyo. ²³ Pamene Yehova anakutumani imwe kuchoka ku Kadeshi Barnea na kuti, 'yendani pamwamba na kunkala nayo malo yamene ine nakupasani imwe; koma munapandukila mosusana na malamulo ya Yehova Mulungu wanu, ndiponso simunakulupilile kapena kunvela ku mau yake. ²⁴ Imwe mwankala wopandukila mosusana na Yehova kuchoka pa siku yamene ninakuzibani. ²⁵ Ninagona cha menso yanga pansi pasogolo pa Yehova ayo masiku fote na usiku uli fote, chifukwa anakamba nakuti azakuonongani imwe. ²⁶ Ninapempela kwa Yehova nakuti, 'Imwe Ambuye Yehova, musaonenge banthu banu kapena cholowa chamene imwe mwachiombola kupitila mu ukulu wanu, chamene imwe mwachibwelesa kuchoka ku Igputo na kwanja kwa mpavu. ²⁷ Itanilani kunzeli zanu bakapolo banu Abrahamu, Isaki, na Yakobo; musalangane kuyuma mutima kwa aba banthu, kapena kuipa kwawo, kapena pa uchimo wawo, ²⁸ kuti malo kuchoka kwamene imwe munatibwelesa ife yangakambe kuti, "Chifukwa Yehova sanali kukwanisa kuti ababwelese mu malo yamene analonjeza beve, ndipo chifukwa anabazonda, ababwelesa beve kuti abapaye beve

mu chipululu." ²⁹ Koma nibanthu banu ndipo choloba chanu, bamene munabwelesa kuchoka kupitila mu ukulu wa mpavu zanu na kuonesela kwa mpavu zanu.'

Chapter 10

¹ Pali ija ntawi Yehova anakamba naine, 'Useme yabili mapilisi ya myala monga yoyamba, na kubwela kwa ine pa lupili, na kupanga likasa ya nkuni. ² Nizalemba pa mapilisi mau yamene yanali pa yoyamba mapilisi yamene unapwanya, ndipo uzayafaka mu likasa.' ³ Ndipo ninapanga likasa ya mutengo wa mtete, na kusema yabili mapilisi ya myala monga yoyamba, ndipo ninayenda pamwamba pa lupili, nili na yabili mapilisi mumanja yanga. ⁴ Analemba pa mapilisi, monga malembendwe yapoyamba, yali teni malamulo yamene Yehova anakamba kuli imwe pa lupili kuchoka mukati mwa mulilo pa siku ya kusonkana; ndipo Yehova anayapasa kwa ine. ⁵ Ninapindamuka na kubwela pansi kuchoka palupili, na kufaka mapilisi mu likasa yamene ninapanga; paja yalipo, monga Yehova alamulila." ⁶ (Bathu ba Israeli banayenda kuchoka ku Beeroth Bene Jaakan kupita ku Mosera. Kwamene kuja Aroni anamwalila, kwamene kuja anashikiwa; Eleazar, mwana wake mwamuna, anatumikila monga wansembe mumalo yake. ⁷ Kuchokela kuja banayenda ku Gudgoda, na kuchoka ku Gudgoda kupita ku Jotbata, malo ya misinje yamanzi. ⁸ Kuchokela pali ija ntawi Yehova anasanka mutundu wa Levi kuti utenge likasa ya chipangano cha Yehova, kuimilila pamenso ya Yehova ku mutumikila, na kudalisa banthu mu zina yake, monga lelo. ⁹ Ndiponso Levi alibe gawo kapena cholowa mu malo pamozi na babale bake; Yehova ndiye cholowa chake, monga Yehova Mulungu wako akambila kuli eve.) ¹⁰ Ninankala pa lupili monga paja pantawi yoyamba, masiku yali fote na usiku uli fote. Yehova ananvela kwa ine pali ija ntawi futi; Yehova sanafune kuti akuonongeni imwe. ¹¹ Yehova anakamba kuli ine nakuti, 'Nyamuka, yenda pasogolo pa banthu kuti ubasogolele beve munjila yawo; bazayenda mukati na kunkala nayo malo yamene ninalapila kwa makolo kuti nipasa kuli beve.' ¹² Manje, Israeli, nichani chamene Yehova Mulungu wanu amafuna kuli imwe, kuchosako kuyopa Yehova Mulungu wanu, kuyenda muli zonse njila zake, kumukonda, na kumulambila Yehova Mulungu wanu na wonse mutima wanu na wonse umoyo wanu, ¹³ kusunga malamulo ya Yehova, na malemba, yamene nikulamulilani imwe lelo pa zabwino zanu? ¹⁴ Onani, kuli Yehova Mulungu wanu kumwamba ni kwake na kumwamba kwa kumwamba, na ziko yapansi, na vonse vilimo. ¹⁵ Yehova eka anatengamo kukondwela mu makolo yanu kuti abakonde, ndipo anabasanka, namibadwe yawo, pambuyo pawo, kuchila aliwonse winangu munthu, monga amachitila lelo. ¹⁶ Ndiponso dulani kungu ya mutima wanu, ndipo musayumise miskosi yanu. ¹⁷ Chifukwa Yehova Mulungu wanu, ni Mulungu wa milungu na Mbuye wa mbuye, Mulungu wamukulu, wampavu ndiponso wopambana, wamene sasamalila aliyense ndipo samatenga zaupupu. ¹⁸ Amawelizila bwino bana bamasiye na wofedwa, ndipo amalangiza chikondi kwa mulendo pakumupasa vakudya na vovala. ¹⁹ Ndiponso kondani mulendo; chifukwa munali balendo mu ziko ya Igputo. ²⁰ Muzayopa Yehova Mulungu wanu; Yeve muzamulambila. Kuli yeve muzagwililila, na pali zina yake muzalumbila. ²¹ Iye ndiye kutamanda kwanu, ndipo ni Mulungu wanu, wamene wachita kwa imwe ivi vikulu na vopambana vintu, vamene menso yanu yaona. ²² Makolo yanu yanayenda ku Igputo monga bali sevirte banthu; manje Yehova Mulungu wanu akupangani imwe bambili monga nyenyezi zakumwamba.

Chapter 11

¹ Ndiponso muzakonda Yehova Mulungu wanu na lonse kusunga malangizo, malemba, malamulo na malamulo yake. ² Zibani kuti sinikamba na bana banu, bamene sibanazibe kapena banaonapo chilango cha Yehova Mulungu wanu, ukulu wake, mpavu za manja yake, kapena kotambuluka kwanja kwake, ³ zioneselo na zochita zamene anachita mukati mwa Igputo kuli Farao, mfumu ya Igputo, na kuli bonse ba mu ziko. ⁴ Ndipo sibanaone zamene anachita kuba nkondo yaku Igputo, kuli bakavalo bawo kapena kuli magaleta yawo, mwamene anapangila manzi yamu nyanja ya mabango yanabatenga beve pamene bana kukakamilani bambuyo panu, na mwanene Yehova anabaononga beve kufikila lelo, ⁵ kapena zamene anakuchitilani imwe mu chipululu kufikila pamene munabwela paliyane malo. ⁶ Sibanaone zamene Yehova anachita kuli Dathani na kuli Abiramu, bana bamuna ba Reubeni, mwamene ziko yapansi inasegula kamwa kake na kubamela beve, mabanja yawo, misasa yawo, na chonse chamoyo chamene chinabakonka beve, mukati mwa bonse ba Israeli. ⁷ Koma menso yanu yaona zonse zikulu nchito ya Yehova zamene anachita. ⁸ Mwaichi sungani yonse malamulo yamene nikulamulilani imwe lelo, kuti munkale wolimba, na kuyenda mukati na kunkala nayo malo kwamene muyenda kuja kuti munkale nayo, ⁹ na kuti masiku yanu yayende pasogolo mu malo yamene Yehova analumbila kuli batate banu kubapasa beve na kuli mibadwe yawo, malo yochosa mukaka na uchi. ¹⁰ Chifukwa malo, kwamene imwe muyenda mukati kunkala nayo, siyali monga malo yaku Igputo, kuchoka kwamene imwe munachoka, kwamene munashanga mbeu na kutilila namendo yanu, monga munda wa masamba; ¹¹ koma malo, yamene muyendamo kunkala yanu, nimalo ya mapili na migodi, ndipo yakumwa manzi ya mvula ya kumwamba, ¹² malo yamene Yehova Mulungu wanu ayasunga; menso ya Yehova Mulungu wanu yali pamene apo, kuchokela mukuyamba kwa chaka kufikila mukusila kwa chaka. ¹³ Chizachitika, ngati muzanvesesa kuli malamulo yanga yamene nikulamulilani imwe lelo, kukonda Yehova Mulungu wanu na kumusebenzela na mutima wanu bonse na umoyo wanu bonse, ¹⁴ kuti nikakupaseni imwe mvula ya mumalo mwanu muntawi yake, mvula yakudala na mvula yamanje, kuti muyende kubwelesa pamozi mbeu zanu, vinyu wanu wasopano, na mafuta yanu. ¹⁵ Nizapasa mauzu mininda yanu ku ng'ombe, ndipo muzadya na kukuta. ¹⁶ Pelekani nzelu kuli imwe mweka kuti mutima wanu usanyengedwe, na kupindamukila kumbali na kulambila milungu inangu na kugwada pansu kuli yeve; ¹⁷ kuti ukali wa Yehova usanyamukile mukususana naimwe; na kuti asavale kumwamba kuti kusankale mvula, na kuti malo yasabale zipaso zake, nakuti imwe musaonongeke mwamusanga kuchokamo mu malo yabwino yamene Yehova akupasani imwe. ¹⁸ Ndiponso ikani pamwamba aya mau yanga mu mutima na muumoyo wanu, yamangeni monga chonesela mu manja mwanu, ndiponso lekani yankale monga pasogolo pakati pa menso yanu. ¹⁹ Muzayapunzisa kuli bana banu na kuyakambapo pamene mwankala pansu munyumba yanu, napamene muyenda munjila, napamene mugona, na pamene muuka. ²⁰ Muzayalemba aya pa poonekela pa makomo ya nyumba yanu na pongenela pa minzi yanu, ²¹ kuti masiku yanu na masiku ya bana banu yachuluke mu malo yamene Yehova analumbila kuli makolo banu kubapasa beve monga kumwamba kuli pamwamba kupambana ziko lapansi. ²² Ngati muzasamala kusunga yonse aya malamulo yamene nikulamulilani imwe, monga mwakuyachita, kukonda Yehova Mulungu wanu, kuyenda munjila zonse zake, na kungilila kuli eve, ²³ ndipo Yehova azachosapo yonse aya maziko kuchoka pasogolo panu, ndipo muzatenga maziko yakulu ndipo yampavu kuchila imwe mweka. ²⁴ Paliponse pamalo pamene pazi ya mendo yanu yazadyaka yazankala yanu; kuchokela mu chipululu panka ku Lebanoni, kuchokela ku mumana, mumana wa Euphrates, kufikila ku mazulo kwa nyanja izankala malile yanu. ²⁵ Kulibe munthu azkwanisa kuimilila pasogolo panu. Yehova Mulungu wanu azaika manta yanu na kuyopewa kwanu pali yonse malo yamene muzandyakapo, mwamene akambila kuli imwe. ²⁶ Onani, Naika pasogolo panu lelo daliso na tembelelo: ²⁷ daliso, ngati imwe muzanvelela malamulo ya Yehova Mulungu wanu yamene nikulamulilani imwe lelo, ²⁸ ndipo tembelelo, ngati simuzasunga malamulo ya Yehova Mulungu wanu, koma pindamukani kuchoka ku njila yamene nikulamulilani imwe lelo, kuchoka pambuyo pa milungu inangu yamene simunaizibe. ²⁹ Chizachitika, pamene Yehova Mulungu wanu abelesa imwe mu malo yamene muyenda mukutenga, kuti muzaika daliso pa phili ya Gerizim, ndipo tembelelo pa pili ya Ebal. ³⁰ Naga siyapitilila Yodani, kumazulo kwa kunjila yaku mazulo, mu malo ya makanani bamene bankala mu Arabah, pamwamba posusana na Giugo, kumbali ya mapepe ya Moreh? ³¹ Chifukwa muli mukujumpila ku Yodani kuyenda nu kutenga malo yamene Yehova Mulungu wanu akupasani imwe, ndiponso muzayatenga na kunkala yanu. ³² Muzasunga yonse malemba na malamulo yamene yaika pasogolo panu lelo.

Chapter 12

¹ Aya ndiyo malemba na malamulo yamene imwe muzasunga mu malo yamene Yehova, Mulungu wa batate banu, akupasani imwe kunkankala yanu, yonse masiku yamene muzankala paziko yapansi. ² Imwe mwachilungamo muzaonga yonse malo kwamene maziko yamene imwe muzayatenga yanalambila yawo milungu, pamwamba pa mapili, pa chulu, na pansu pa chilichonse choifilila chimutengo. ³ Mufunika kugwesa pansu maguwa yawo, kuononga kunkala tung'ono tung'ono maziko ya myala, na kushoka Asherah yogwilila. Mufunika kujuba pansu vosema woonesela va milungu yawo na kuononga zina yawo kuchoka muli yaja malo. ⁴ Simuzalambila Yehova Mulungu wanu monga vija. ⁵ Koma kumalo kwamene Yehova Mulungu wanu azasanka kuchoka kuli yonse mitundu kuika zina yake, yamene ayo yazankala malo yamene ankala, ndipo niye kwamene imwe muzayenda. ⁶ Nikwamene kuja kwamene muzabwelesa nsembe yoshoka, chopeleka, cha kumi, na chopeleka chopasidwa na manja yanu, chopeleka chanu chakulumbila, chopeleka chanu chozifunila, na yoyamba mwa ng'ombe na zobeta zanu. ⁷ Nikwamene kuja kwamene imwe muzadya pasogolo pa Yehova Mulungu wanu na kusangalala muli vili vonse vamene muzaikapo manja yanu, imwe na bamunyumba yanu, kwamene Yehova Mulungu wanu akudalisani imwe. ⁸ Simuzachita vonse vintu vamene tili kuchita kuno lelo; manje aliyense achita chilichonse chili bwino mumenso yake; ⁹ chifukwa simunabwele ku mupumulo, ku cholowa chamene Yehova Mulungu wanu akupasani imwe. ¹⁰ Koma ngati mwayenda kuja ku Yodani na kunkala mu malo ya Yehova Mulungu wanu alengesa imwe kuti mutenge, ndipo azakupasani imwe mupumulo kuchoka kuli bonse badani banu okuzungulilani, kuti munkale ochingilizidwa. ¹¹ Ndipo ku malo yamene Yehova Mulungu wanu azasanka kupanga zina yake kunkala kwamene uko-uko muzaleta vili vonse nikulamulilani imwe: chopeleka choshoka chanu, chopeleka chanu, chakumi chanu, na chopeleka chopasidwa na manja yanu, na chosanka copeleka cha kulambila chamene muzalambila kwa Yehova. ¹² Muzasangala basogolo pa Yehova Mulungu wanu-imwe, bana banu bamuna, bana banu bakazi, banchito banu bamuna, banchito banu bakazi, na ma Levi bamene bali mukati mwa geti yanu, chifukwa alibemo gawo kapena cholowa mukati mwaimwe. ¹³ Pelekani kunvesesa kwa imwe mweka kuti musapase cha chopeleka chanu choshoka pa yali yonse malo yamene muona; ¹⁴ koma ni pali malo yamene Yehova azasanka mwa umozi mutundu wamene uzapeleka chopeleka choshoka chanu, ndipo uko muzachita vilivonse vamene nikulamulilani imwe. ¹⁵ Komanso, mungapaye na kudya nyama mukati monse mwa mageti yanu, monga mwamene mufunila, kulandila madaliso ya Yehova Mulungu wanu pali vonse vamene akupasani imwe; osayela na oyela banthu bonse bangadye, nyama monga Gazelle na mbelele. ¹⁶ Koma simuzadya magari; muzayatila paziko yapansi monga manzi. ¹⁷ Imwe simungadye mukati mwa mageti yanu kuchoka ku chakumi chanu chambeu, vinyu yanu yamanje, mafuta yanu, kapena yoyamba mwa zobeta zanu; ndiponso simungadye iliyonse mwa nyama imwe mwaipasa pamozi na kulumbila kwanu kwamene mwapanga, kapena mwa kupeleka kwa kufuna kwanu, kapena kuja kwa chopeleka imwe mupeleka na manja yanu. ¹⁸ Koma, muzadya ivo pasogolo pa Yehova Mulungu wanu mu malo yamene Yehova Mulungu wanu azasanka-you, bana banu bamuna, bana banu bakazi, banchito banu bamuna, banchito banu bakazi, na ma Levi bamene bali muka mwa ma geti yanu; muzasangalala basogolo pa Yehova pali vili vonse vamene muyaikapo manja yanu. ¹⁹ Pelekani nzelu kwa imwe mweka kuti musakane mu Levi ngati chabe muli na moyo mu malo yanu. ²⁰ Pamene Yehova Mulungu wanu akulisa malile yanu, monga mwamene analonjezela kuli imwe, ndipo imwe muka, 'Nizadya tupi, 'chifukwa chakufuna kwanu kudya nyama, mungadye nyama, monga moyo wanu ufunila. ²¹ Koma ngati malo yamene Yehova Mulungu wanu ayasanka kuika zina yake yali patali kuchoka kuli imwe, ndipo muzapaya zinangu mwa nyama zanu na zobeta zanu zamene Yehova anakupasani imwe, monga mwamene nikulamulilani imwe; mungadye mukati mwa mageti yanu, monga moyo wanu ufunila. ²² Monga Gazelle na mbelele zidyewa, ndipo mungadye kwa iyo; wasayela na oyela banthu bangadye chimozimozi. ²³ Koma nkalani oziba kuti musamwe magari, chifukwa magari ni umoyo; siuzadya umoyo pamozi na nyama. ²⁴ Iwe siuzadya icho; uzataya icho panja pa ziko yapansi monga manzi. ²⁵ Iwe siuzadya icho, kuti ziyende bwino kwa iwe, na bana pambuyo pako, pamene iwe wachita chamene chili bwino pa menso ya Yehova. ²⁶ Koma vinthu vamene vake va Yehova vamene imwe mulinavo na kupasa mwa kulumbila kwanu-tengani ivi vintu na kuyenda ku maloyamene Yehova ayasanka. ²⁷ Uko muzapeleka chopeleka choshoka, nyama na magari, pa guwa ya Yehova Mulungu wanu; magari ya chopeleka chanu yazatilidwa kuchoka pa guwa ya Yehova Mulungu wanu, ndipo imwe muzadya tupi. ²⁸ Sungani na kunvela kuli yonse mau yamene nikulamulilani imwe, kuti ziyende bwino kwa imwe na kuli bana bambuyo panu kwamuyayaya, pamene mwachita zamene zili bwino na zolungama pa menso ya Yehova Mulungu wanu. ²⁹ Pamene Yehova Mulungu wanu ajuba ma ziko kuchoka basogolo panu, mukayenda mukati kukatenga ivo, na kuvitenga ivo, na kunkala mu malo yawo, ³⁰ pelekani nzelu kwa imwe mweka kuti musagwilidye kukonka beve, pambuyo bakaonongeka kuchoka pasogolo panu-kugwilidwa mu kufunafuna

milungu yawo, mu kufunsa, 'Bwanji aya ma ziko yalambila milungu yawo? Nizachita chimozi.'³¹ Simuzalambila Yehova Mulungu wanu muli iyo njila, chifukwa chili chonse chamene chili chonyasa kwa Yehova, vintu vamene azonda-bavichita ivi na milungu yawo; bamashoka ngankale bana bawo bamuna ba bana bawo bakazi mu mililo kwa milungu yawo.³² Chili chonse chamene nikulamulilani, sungani ivo. Musaonjezelepo kapena kuchosapo.

Chapter 13

¹ Ngati kuli wanyamuka mwaimwe muneneli kapena wolota maloto, na kukupasani imwe choonesela kapena chodabwisa, ² ndipo ngati choonesela kapena chodabwisa chabwela, monga iye anakambila kuli imwe na kuti, 'Tiyeni tiyende pambuyo pa milungu inangu, yamene simunaizibe, ndipo tiyeni tiilambile,' ³ musanvelele ku mau ya uyo muneneli, kapena uyo olota maloto; chifukwa Yehova Mulungu wanu akuyesani imwe kuziba ngati imwe mumukonda Yehova Mulungu wanu na mutima wanu wonse na umoyo wanu wonse. ⁴ Muzayenda pambuyo pa Yehova Mulungu wanu, kumulemeke iye, kusunga malamulo yake, na kunvela mau yake, ndipo muzamulambila na kugwililila kuli eve. ⁵ Uyo muneneli kapena uyo olota malotoazikidwa ku infa, chifukwa akamba kusanvelela mosusana na Yehova Mulungu wanu, wamene anakuchosani kuchoka mu ziko ya Igputo, ndipo anakuombolani imwe kuchoka mu nyumba ya ukapolo. Uyo muneneli afuna kukuchosani imwe kuchoka munjila yamene Yehova Mulungu wanu analamulila imwe kuyendamo. koma ikani kutali zoipa kuchoka pakati panu. ⁶ Nanga ngati mubale wako, mwana mwamuna wa amai bako, kapena mwana wako mwamuna, kapena mwana wako mukazi, kapena mukazi wako wapachifuba, kapena munzako wamene ali kuli iwe monga umoyo wako, mobisika akakunyengelela iwe nakuti, 'Tiye ndipo tilambile milungu inangu yamene siunazibe, kapena iwe kapena makolo bako- ⁷ iliyonse milungu ya banthu yamene yokuzungulilani, pafupi naimwe, kapena patali naimwe, kuchoka kumoji kosilizila ziko lapansi na kufika kwina kosilizila ziko yapansi.' ⁸ Simufunika kupasa kuli eve kapena kunvela kuli eve, ndipo simufunika kulola menso yanu kumunvelela chifundo, ndiponso simufunika kumulekelela kapena kumuchingiliza eve. ⁹ Koma, imwe mufunika kumupaya; manja yanu yafunika kunkala yoyamba kufaka eve kuifya, na bambuyo pake manja ya bonse banthu. ¹⁰ Muzamulasa eve mpaka infa na myala, chifukwa ayesa kukuchosani imwe kuchoka kwa Yehova Mulungu wanu, wamene anakuchosani imwe ku ziko ya Igputo, kuchoka kunyumba ya ukapolo. ¹¹ Bonse ba Israeli bazanvela na kuyopa, ndipo sibazapitiliza kuchita monga ichi chintu chosayela mukati mwanu. ¹² Ngati mwanvela aliyense akuti pali umozi mwa minzi yanu, kuti Yehova Mulungu wanu akupasani kuti munkalemo: ¹³ Benangu woipa banthu bayenda kuchoka mukati mwanu na kuchosa mibadwe ya minzi yawo na kuti, 'Lekani tiyende na kulambila milungu inangu yamene simuziba.' ¹⁴ Ndipo muzayesa chizibiso, kupanga kufuna, na kufunisisa kwabwino. Koma mukapeza kuti nizoona na kuziba kuti icho chonyansa chinthu chachitika mukati mwanu, ndipo muzatenga chisanzo. ¹⁵ Imwe zoona mufunika kuononga wonkalamo ba muja mumunzi na lupanga, kuonongelatu na banthu bonse bamene balimo, na vonse vibeto, na lupanga. ¹⁶ Muzabwelesa pamozi vonse voonongeka kuchoka uko kufika mukati mwa njila na kushoka mizinda, na pamozi navoonongeka vake- chifukwa cha Yehova Mulungu wanu. muzinda uzankala choononga muyayaya; siifunika kumangidwa futi. ¹⁷ Palibe chimodzi mwazinthu zoyikidwa kuti ziwonongedwe siziyenera kukhala m'manja mwanu. Izi zikhale choncho, kuti Yehova atembenuke kuchoka mkwiyo wake woyaka mkwiyo, akuchitireni chifundo ndi kukuchitirani chifundo ndi kukuchulukitsani monga analumbirira makolo anu. ¹⁸ Azichita izi chifukwa chakuti mumvera mawu a Yehova Mulungu wanu, kusunga malamulo ake onse amene ndikukupatsani lero, ndi kuchita zoyenera pamaso pa Yehova Mulungu wanu.

Chapter 14

¹ Ndimwe banthu ba Yehova Mulungu wanu. Musaziguwe mweka, kapenga kugela mbali iliyonse ya pamenso panu pa bakufa. ² Chifukwa ndimwe ziko yopatulika kwa Yehova Mulungu wanu, ndipo Yehova akusankani imwe kunkala banthu bake, kuchila banthu bonse bamene bali pa ziko lapansi. ³ Simufunika kudya chili chonse chosayela chintu. ⁴ Izi ndiye nyama zamene mungadye: n'gombe, nk'hosa, na mbuzi, ⁵ mbawala, gazelle, roebuck, mbuzi yamusanga, na nkumba, na antelope, na zapapili nkosa. ⁶ Mungadye iliyonse nyama yamene igabanisa vibodo, ndiye kuti, yamene ili na vibodo vogabikana pabili, ndipo yamene isheta masamba. ⁷ Komanso, simufunika kudya nyama zinangu zamene zikudya masamba kapena zamene zili na vibodo vogabanikana pabili: Ngamila, kalulu, na mbila; chifukwa zimasheta masamba koma sizogabanisana vibodo, nizosayela kuli imwe. ⁸ Nkumba niyosayela kuli imwe nayonso chifukwa niyogabanikana vibodo koma siisheta visamba; niyosayela kuli imwe. Osadya nyama ya nkumba, ndipo musagwila chitumbia chake. ⁹ Muli ivi vinthu vamene vili mumanzi mungadye: vamene vili na minga na mamba; ¹⁰ koma vamene vilibe minga na mamba simufunika kudya; nivosayela kuli imwe. ¹¹ Mutha kudya mbalame zonse zoyera. ¹² Koma izi ndi mbalame zomwe simuyenera kudya: chiwombankhanga, chiwombankhanga, ntchentche, ¹³ mphamba wofiira ndi mphamba wakuda, mtundu uliwonse wa mphamba. ¹⁴ Musadye mtundu uliwonse wa khwangwala, ¹⁵ nthiwatiwa, ndi kabawi usiku, mbalame zam'madzi, mtundu uliwonse wa nk'hono, ¹⁶ kadzidzi, kadzidzi wamkulu, kadzidzi woyera, ¹⁷ vuwo, nkhanu, kanyama kena. ¹⁸ Simuyenera kudya dokowe, mtundu uliwonse wa chimeza, hoopoe, ndi mileme. ¹⁹ Zinthu zonse zamapiko ndi zothamanga ndi zodetsedwa kwa inu. siziyenera kudyedwa. ²⁰ Mutha kudya zouluka zonse zoyera. ²¹ Simufunika kudya chili chonse chamene chazifela cheka; mungachipase kuli mulendo wamene wamene ali mu minzi yanu, kuti angaidye; kapena mungaigulise kuli mulendo. Chifukwa ndimwe ziko yamene ili yopatulika kwa Yehova Mulungu wanu. Simuzabilisa mbuzi ing'ono yamene namukaka wa mai wake. ²² Mufunika zoona kupeleka chakumi cha zobadwa ku mbeu zanu, chamene chichoka mumunda wanu chaka pambuyo pa chaka. ²³ Mufunika kudya pasogolo pa Yehova Mulungu wanu, mu malo yamene azasanka monga kachisi yake, chakumi cha tiligu yanu, vinyu wanu wasopano, na mafuta yanu, na yoyamba mwa vobeta vanu; kuti mupunzile ntawi zonse kulemekeza Yehova Mulungu wanu. ²⁴ Ngati ulendo wanu niutalikuti kapena simungakwanise kutenga, chifukwa malo yamene Yehova Mulungu wanu azasanka monga kachisi yake yali patali kuchoka kuli imwe, ndipo, pamene Yehova Mulungu akudalisani, ²⁵ muzachinja chopeleka mu ndalama, mangani ndalama mumanja yanu, na kuyenda ku malo yamene Yehova Mulungu wanu azasanka. ²⁶ Kwamene uko muzasebenzesa ndalama pa vilivonse vamene mufuna: ng'ombe, nkosa, vinyu kapena vikali, kapena vilivonse vamene mufuna. Ndipo muzadya uko pasogolo pa Yehova Mulungu wanu na kusangala, imwe na nyumba yanu. ²⁷ Mu Levi bamene bali mukati mwanu- musamukane iye, chifukwa alibe mbali kapela cholowa pamozi na imwe. ²⁸ Pa kusila kwa zilizonse zaka zitatu muzabwelesa zonse zakumi zakukolola kwanu muchamene icho chaka, ndipo muzasungila mukati mwa makomo yanu; ²⁹ nama Levi, chifukwa alibe gawo kapena cholowa mwa imwe, na mulendo, na mwamuna wosabala, na mukazi wofedwa wamene ali mukati mwa mageti yanu, azabwela na kudya na kukuta. Chitani ichi kuti Yehova Mulungu wanu akudaliseni muli iliyonse nchito yamanja yanu.

Chapter 15

¹ Pa kusila kwa zaka zili seveni, mufunika kuchosapo nkongole. ² Iyi ndiye njila kuomboledwa: Aliyense wankongile azachosapo chija chamene anabweleka kuli munzake wapafupi; sazafunsa kuchokela kuli munzake wapafupi kapena mubale wake chifukwa kuchosapo kwa Yehova kwa kambidwa. ³ Kuchokela kuli mulendo mungafunsepo; koma chilichonse cha imwe ngati chili na mubale wanu kwanja kwanu kufunika kulekelako. ⁴ Komanso, sikufunika kunkala osaukwa mwaimwe (chifukwa Yehova zoona azakudalisa imwe mu malo yamene akupasani imwe munga cholowa kuti munkale nacho), ⁵ ngati chabe mosamala munvela kuli mau ya Yehova Mulungu wanu, kusunga yonse aya malamulo yamene nikulamulilani imwe lelo. ⁶ Chifukwa Yehova Mulungu wanu azakudalisani imwe, munga analonjezakwa imwe; muzakongolesa yambili maziko, koma imwe simuzakongola; muzalamulila yambili maziko, koma sibazakulamulilani imwe. ⁷ Ngati kuli wina osauka mwaimwe, umozi mwa babale bako, mukati mwa mageti yanu mu malo yanu yamene Yehova Mulungu wanu akupasani imwe, simufunika kulimbisa mitima yanu kapena kuvala manja yanu kuchoka kwa osauka mubale; ⁸ koma mufunika zoona kusegula manja yanu kuli eve nazoona kumukongolesa zokwanila pa zofuna zake. ⁹ Nkalani ochonjela osankala nayoipa maganizo mu mutima wanu, nakuti, 'Muchaka cha namba seveni, chaka chochosa, chili pafupi,' kuti imwe musankale bakaso mu nkani ya osauka mubale wanu na kusamupasa ive kalikonse; afunika kulilila kwa Yehova chifukwa chanu, ndipo uzankala uchimo kwa imwe. ¹⁰ Mufunika zoona kumupasa, ndipo mutima wanu usankale wopepa pamene mukamupasa eve, chifukwa kubwezela kwa ichi Yehova Mulungu wanu azakudalisani imwe muli iliyonse nchito yanu na muli vili vonse vamene muikapo manja yanu. ¹¹ Chifukwa osauka sibazaleka kunkala mu ziko; mwaichi nikulamulilani imwe nakuti, 'mufunika zoona kusegula manja yanu kwa mubale wanu, kuofuna banu, na kuosauka mu malo mwanu.' ¹² Ngati mubale wako, mwamuna wachi Eberi, kapena mukazi wachi Eberi, aguliswa kwa imwe na kukusebenzela mu zaka zili sikisi, ndipo muchaka cha namba seveni ufunika kumuleka kuti ayende wakayeke kuchoka kuli imwe. ¹³ Ndipo mukamulekelela kuyenda wakayeke kuchoka kuli imwe, simufunika kuti ayende manja-manja. ¹⁴ Mufunika mofunikila kumupasa eve kuchoka ng'ombe zanu, kuchoka kuzantaka zanu, na kuchoka ku chosungilamo waini. Munga Yehova Mulungu wanu akudalisani imwe, mufunika kupasa kwa eve. ¹⁵ Mufunika kukumbukila kuti munali bakapolo mu ziko ya Igputo, ndipo Yehova Mulungu wanu anakuombolani imwe; ndiponso nikulamulilani imwe lelo kuchita ichi. ¹⁶ Chizachitika kuti ngati akuuzani imwe, 'Sinizayenda kuchoka kuli imwe,' chifukwa akukondani imwe na nyumba yanu, ndipo chifukwa chakuti alibwino pamozi naimwe, ¹⁷ ndipo mufunika kutenga mbila na kuiponyela kupitila kukwatu pa komo yanu, ndipo azankala kapolo wanu umoyo wake bonse. Mufunika kuchita chimiozi-mozi na wanchito wanu mukazi. ¹⁸ Sichifunika kuoneka cholimba kuli imwe kuleka eve kuti ayende wamutendele kuchoka kuli imwe, chifukwa akusebenzelani pa zaka zili sikisi na kupasa kabili mutengo wa muntu wobweleka. Yehova Mulungu wanu azakudalisani muli vilivonse vamene muchita. ¹⁹ Bonse bana woyamba bamuna mu zobeta zanu na zochema zanu mufunika kuzipatula kuli Yehova Mulungu wanu. Simuzagwila iliyonse nchito na zoyamba zobadwa ya zobeta zanu, kapena kusebenzesa zobamba zoyamba zochema zanu. ²⁰ Mufunika kudya zobadwa zoyamba pasogolo pa Yehova chaka na chaka mu malo yamene Yehova azasanka, imwe na bamunyumba banu. ²¹ Ngati ili naulema ulibonse - mwachisanzo, ngati niyolemala kapena yosapenya, ili naulema ulibonse - simufunika kuipeleka kwa Yehova Mulungu wanu. ²² Muzaidya mukati mwa mageti yanu; wosayela na woyela banthu pamozi bafunika kudya, munga mwamene mungadyele gazelle kapena mbawale. ²³ Koma simufunika chabe kudya magari; mufunika kutila magari yake panja pa doti munga manzi.

Chapter 16

¹ Sungani mwezi wa Abibu, na kusungila Pasika ya Yehovah Mulungu wanu, pakuti mu mwezi wa Abibu Yehovah Mulungu wanu anakutululani kuchoka mu Egypto usiku. ² Muzapeleka nsembe ya Pasika kuli Yehovah Mulungu wanu pamodzi na nkosa na ng'ombe mu malo yamene Yehovah azasanka ngati malo yake opatulika. ³ Simuzadya mukate wopanda chotupisa; Masiku asanu ndi yabili muzadya mukate wopanda chotupisa, mukate wachisautso; chifukwa imwe munackokela mu malo mwa Egypto mwachangu. Chitani izi masiku yanu yonse ya umoyo wanu pakuti mukakubukile siku pamene munachokela mu malo ya Egypto. ⁴ Yisiti isaoneke pakati panu mumalo yanuonse masiku asanu na yabili; kapena nyama yozipeleka nsembe mazulo pasiku yoyamba isakhale kufikila naku mawa. ⁵ ⁶ Musapeleke nsembe ya pasika mu mzinda wanu ulionse wamene Yehovah Mulungu wanu akupasani. M'malo mwake, pelekani nsembe pamalo yamene Yehovah Mulungu wanu azasankha monga malo yake opatulika. Mukapeleka nsembe ya pasika kuma zulo pamene zuba ikulowa, pa nthawi ya chaka chamene munachoka ku Egypto. ⁷ Muyenela kuyishoka na kuyidya pamalo yamene Yehovah Mulungu azasankha; m'mawa muzatembenuka na kupita kuma hema yanu. ⁸ Masiku asanu ndi imodzi muzadya mukate wopanda chotupisa; pasiku ya chisanu na chibili muzankhala na musokano waukulu wa Yehovah Mulungu wanu; pasiku yamene iyi simuyenekela kugwila nchito iliyonse. ⁹ Mubelenge masabata asanu ndi abili; kuyambila pamene munayamba kukweza chikwakwa ku tirigu wosasunthika muyenela kubelenga milungu isanu na ibili. ¹⁰ Muzasunga chikondwelelo cha masabata cha Yehovah Mulungu wanu ndi chopeleka chaufulu chochokela mumanja yanu chimene mupeleka. Monga mwamene Yehovah Mulungu wako akudalisani. ¹¹ Muzakondwela pamanso pa Yehovah Mulungu wako- iwe, mwana wako mwamuna, mwana wako mkazi, kapolo wako mwamuna, kapolo wako mkazi, Mlevi wamene ali mkati mwa zipata za mzinda wanu, mlendo, mwana wamasiye, na mkazi wamasiye wamene ali pakati panu, pamalo yamene Yehovah Mulungu wanu azasankha ankhale malo yake opatulika. ¹² Uzakumbukila kuti munali kapolo ku Egypto; muyenela kuona na kuchita maudindo aya. ¹³ ¹⁴ Muzasunga chikondwelelo cha misasa mumasiku yali seveni pambuyo mukasonkana mu kukolola kuchoka na kuchokela mu mosungila waini yanu. ¹⁴ Uzasangalala pa chikondwelelo chako - Iwe, mwana wako mwamuna, mwana wako mukazi, wanchito wako mwamuna, wanchito wako mukazi, mu Levi, na mulend, na mwana wamasiye, na mukazi wamene ali mukati mwa muzinda wanu. ¹⁵ Masiku yali seveni mufunika kusunga madyelelo ya Yehova Mulungu wanu pa malo yamene Yehova azasanka, chifukwa Yehova Mulungu wanu azakudalisani muli zonse zako za kukolola na zonse ncito za manja yako, nakuti unkale wokondwela maningi. ¹⁶ Masiku yatatu mu chaka bonse bamuna bafunika bazibwela pamenso pa Yehova Mulungu wanu pa malo yamene azasanka: pa chikondwelelo cha buledi yopanda chotupisa, pa chikondwelelo cha masabata, na pachikondwelelo chamisasa. Palibe munthu azaonekela pamenso ya Yehova alibe kanthu; ¹⁷ Mumalo mwake, aliyense apeleke vamene akwanisa, kuti muzibe ma daliso yamene Yehova Mulungu wanu akupasani. ¹⁸ Mufunika kupanga boweluza na oyanganila mukati monse mwa zipata za muzinda wanu wamene Yehova Mulungu wanu akupasani; azatengewa kuchokela ku mitundu yonse yanu, ndipo bafunika kuweluzwa banthu kuweluzwa cholungama. ¹⁹ Osachosa chilungamo mokakamiza; musakondwele kapena kulandila chipupu cha chivimba menso ya banzeli na kupindamula mau ya olungama. ²⁰ Mufunika kukonka chilungamo, pambuyo pa chilungamo cheka, kuti munkale na umoyona kulandila ziko yamene Yehova Mulungu wanu akupasani. ²¹ Simufunika kuzipangila asherah wanu, mutengo uliwonse, pambali pa guwa ya nsembe ya Yehova Mulungu wanu kuti muzipangile mweka. ²² Kapena kuzipangila mweka chipila cha mwala, chamene Yehova Mulungu wanu azonda.

Chapter 17

¹ Musapeleke kuli Yehova Mulungu wanu ng'ombe kapena nkosa yamene ili chilema kapena chilichonse choipa, chifukwa ichi chingankale chonyansa kuli Yehova Mulungu wanu. ² Ngati papezeka pakati panu, mukati mwa mizinda yanu kuti Yehova Mulungu wanu akupasani, mwamuna aliyense kapena mukazi wamene achita choipa pamenso ya Yehova Mulungu wanu na kupwanya chipangano chake, ³ aliyense wamene ayenda muku pembeza milungu inangu na kuigwadila, ngankale zuba, mwezi, kapena chilichonse cha kumwamba - chamene sininalamulile - ⁴ ndipo ngati mwauzidwa pali ichi, kapena mwanvelako pali ichi, ndiye mufunika kufufuza mosamalila. Ngati nizoona ndipo choona kuti icho chonyansa china chitika mu Israeli, ichi ndiye chamene mufunika kuchita. ⁵ Mufunika kubwelesa uyo mwamuna kapena mukazi, wamene achita ichi choipa, kuzipata za mizinda yanu, wamene uyo mwamuna kapena mukazi, ndipo mufunika kumutema myala uyo muntu kuti afe. ⁶ Pakamwa pa mboni zibili, kapena zitatu, wamene apaiwa afunika kupaiwa; koma pa kamwa ya imozi mboni safunika kuikidwa kuinfa. ⁷ Manja ya mboni yafunika kuyamba kumuika kuinfa, ndipo pambuyo pake bonse banthu; ndipo muzachosa choipa pakati panu. ⁸ Pakankhala nkhani yovuta kuti imwe muweruze - mwina funso yakupaya kapena kufa mwangozi, ufulu wa munthu m'modzi na wina, kapena funso mtundu umodzi wamene wachitika, kapena nkhani yamtundu wina, nkhani zosutsana mkati mwa zipata za mzinda wanu- pamene apo mupite kumalo kwamene Yehovah Mulungu wanu azasankha ankhale malo ake opatulika. ⁹ Mupite kwa ansembe, mibadwo za Levi, ku woweruza bamene azankhala alikugwila nchito pa nthawi yamene iyo ; mukabafunse upangili wawo, ndipo azakupasani chigamulo. ¹⁰ Pamene apo muyenela kuchita monga mwamene akukulamulilani, pamalo yamene Yehovah azasankha. Samalani kuchita vonse vamene beve bakuphunzisani imwe. ¹¹ Kusatila malamulo yamene akuphunzisani, osapatuka pa vamene akukuuzani, kuzanja yamanja kapena yamazele. ¹² Aliyense amene achita mozikuza, osamvelela wansembe amene ayimilila kutumikila pamaso pa Yehovah Mulungu wanu, kapena posamvelela woweruza- uja mwamuna azamwalila; muzachosa choipa icho ku Israeli. ¹³ Banthu bonse bayenela kumvela na kuyopa, osachitanso kanthu mozikuza. ¹⁴ Pamene imwe mwabwela ku malo yamene Yehovah Mulungu akupasani imwe, ndipo mukamutenga kunkhala wanu na kukhalamo, 'pameneapo muzakamba kuti, nizaziyikila mfumu, monga mitundu yonse yamene yanizungulukila ine.' ¹⁵ Pamene apo muzaika mfumu azalamulila banthu bamene Yehovah Mulungu wako azamusankila. Muzisankile mweka mfumu wamene ali pakati pa abale wanu. Simungafake mlendo, amene si mbale wako, pali imwe mweka chabe. ¹⁶ Koma eve asaonjezele ma horsi kwake, kapena kuchitisa banthu kubwelela ku Egypto kuti eve aonjezele ma horsi, pakuti Yehovah anakamba kwa imwe kuti, ' Imwe simuzakabwelela munjila ija.' ¹⁷ Eve asazitengele bakazi bambili, kuti mtima wake usachoke. Eve sayenela kuziunjikila siliva na golide wambili. ¹⁸ Pamene ankhala pampando wachifumu wa mfumu wake, eve afunika kuzilembela eka m'buku ya lamulo iyi, kuchokela kulamulo yamene ili pamaso pa nsembe, bamene ba Levi. ¹⁹ Iyi buku ifunika ilina eve, ndipo nakuyibelenga masiku yonse ya umoyo wake, kuti aphunzile kulemekeza Yehovah Mulungu wake, kuti musunge mawu yonse a lamulo iyi na zifanizo. ²⁰ Eve ayenela kuchita izi kuti mtima wake usazikuze pa abale ake, kuti eve asapatuke pa malamulo, kuzanja yamanja kapena yamanzele, kuti eve achuluke masiku yake mu ufumu wake, eve na mbadwo wake pakati pa Israeli.

Chapter 18

¹ Wopeleka nsembe, bamene bali ma Levi, na bonse muntundu wa Levi, sibazankala na gawo kapena kulowa pamozi na Israeli; bafunika kudya chopeleka cha Yehova chopangiwa na mulilo monga cholowa chawo. ² Sibafunika kunkala na kulowa pamozi na babale bawo; Yehova ndiye kulowa kwawo, monga anakambila kuli beve. ³ Iyi ndiye gawo yopasidwa kuli wopeleka nsembe, yopasidwa kuli beve kuchokela ku banthu bamene bapeleka chopeleka, ngankale ingankale ng'ombe kapena nkosa: chipewa, bwavu zibili, na zamukati. ⁴ Zipaso zoyamba za tiligu, ya waini yanuwasonpano, na mafuta yanu, na yoyamba kubadwa ya nkosa zanu, mufunika kumupasa eve. ⁵ Chifukwa Yehova Mulungu wanuamusanka eve kuchoka kuli yonse mitundu kuimilila mu kutumikila muzina ya Yehova, eve na bana bake bamuna muyayaya. ⁶ Ngati mu Levi abwela kuchoka kulikonse ku minzi yanu kuchoka ku monse mu Israeli kuchoka kwamene ankala, nakufunisisa na umoyo wake bonse kubwela kumalo yamene Yehova azasanka, ⁷ ndipo afunika kutumikila muzina ya Yehova Mulungu monga bonse ba bale bake ma Levi bamachita, bamene bamaimilila pasogolo pa Yehova. ⁸ Bafunika kunkala na yolingana ma gawo ya kudya, kuchosako vamene vibwela kuchoka ku zogulisa za cholowa cha banja yake. ⁹ Koma pamene mwabwela mu malo yamene Yehova Mulungu wanu akupasani imwe, simufunika kupunzila kusunga zonyansa za ayo maziko. ¹⁰ Kuja sikufunika kupezeka mwaimwe aliyense wamene apasa mwana wake mwamuna kapena mwana wake mukazi mu mulilo, aliyense wamene asebenzesa kubombeza kapena auza chuma, kapena kubelenga zizindikilo zopezeka mu kapu, kapena achita za unfwiti, ¹¹ bonse waminkwala, aliyense woukisa mizimu, kapene wamene amaponya zakuloza, wamene akamba na mizimu ya bakufa. ¹² Chifukwa aliyenso ochita ivi vintu ni wonyansa kwa Yehova; nichifukwa cha ivi vonyansa kuti Yehova Mulungu wanu abachosamo kuchoka pasogolo panu. ¹³ Mufunika kunkala bakaye pasogolo pa Yehova Mulungu wanu. ¹⁴ Chifukwa aya maziko yamene muzapoka bamanvela kuli awo wochita mansenga na kuombeza; koma monga imwe, Yehova Mulungu wanu sanakuvomelezeni kuchita ivo. ¹⁵ Yehova Mulungu wanu azanyamula kwa imwe muneneli kuchoka mwaimwe, umozi muli babale banu, monga ine. Mufunika kunvela kuli eve. ¹⁶ Ichi ndiye chamene munapempa kuli Yehova Mulungu wanuku Horebu pa siku ya kusonkana, nakuti, 'Lekani ife kuti tisanvele nafuti mau ya Yehova Mulungu watu, kapena kuona uyu mulilo ukulu nafuti, kapena timwalila.' ¹⁷ Yehova anakamba naine, 'Vamene bakamba vili bwino. ¹⁸ Nizanyamula muneneli wawo kuchoka muli mubale wawo, monga chabe iwe. Nizaika mau yanga mukamwa kake, ndipo azakamba kuli beve vonse vamene nizamuuza. ¹⁹ Chizachitika ngati aliyense sazanvela ku mau yanga kuti akamba muzina yanga, nizayafuna kuli eve. ²⁰ Koma muneneli wamene akamba mau mozikuza muzina yanga, mau yamene sininamulile kuti akambe, kapena wamene akamba muzina ya mulungu inangu, wamene uyo muneneli afunika kumwalila.' ²¹ Ichi ndiye chamene mufunika kukamba mumitima mwanu: 'Nanga tizaziba bwanji utenga kapena Yehova akamba?' ²² Imwe muzaziba utenga ngati Yehova akamba pamene muneneli akamba mu zina ya Yehova. Ngati icho chintu sichioneka kapena kuchitika, icho ndicho chintu chamene Yehova sanakambe ndipo muneneli anakamba mozikuza, ndipo simufunika kumuyopa eve.

Chapter 19

¹ Yehova Mulungu wanu akadzawononga mitundu ya anthu, amene Yehova Mulungu wanu akukupatsani dziko lawo, ndi kuwatsata ndikukhala m'mizinda yawo ndi nyumba zawo, ² mudzisankhire mizinda itatu pakati pa dziko lanu, limene Yehova Mulungu wanu adzakupatsani. akukupatsani kuti mukhale anu. ³ Muzimanga msewu ndi kugawa malire atatu a dziko lanu, dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani kuti likhale lanu, kuti aliyense wopha mnzake athawireko. ⁴ Awa ndi malangizo okhudza amene wapha mnzake ndi kuthawa kuchokera kumeneko kuti apulumutse moyo wake — amene amapha mnzake mwangozi osamuda pa nthawi ya ngoziyo. ⁵ Mwachitsanzo, ngati munthu apita kunkhalango ndi mnansi wake kukadula nkhu, nkudula ndi nkhwangwa kudula mtengo, ndipo mutu wa nkhwangwa umadumphira ndi kumenya mnzake ndikupha - ndiye kuti munthuyo ayenera thawirani mumzinda umodzi kuti mupulumutse moyo wake. ⁶ Kupanda kutero wobwezera magazi atha kutsatira amene wapha mnzakeyo, ndipo atakwiya kwambiri amugwira, ngati ndi wautali kwambiri, mumumenye ndi kumupha, ngakhale kuti munthuyo sanayenere kufa, chifukwa sanadane ndi mnzake m'mbuyomu. ⁷ Chifukwa chake ndikukulamulani kuti mudzisankhire mizinda itatu. ⁸ Ngati Yehova Mulungu wanu akulitsa malire anu, monga analumbirira makolo anu, ndi kukupatsani dziko lonse limene analonjezana ndi makolo anu; ⁹ Mukasunga malamulo awa onse kuwachita, amene ndikukulamulani lero; malamulo oti mukonde Yehova Mulungu wanu, ndi kuyenda m'njira zake nthawi zonse, pamenepo mudziwonjezere midzi ina itatu, osawonjezerapo ena atatu. ¹⁰ Chitani izi kuti musakhitse magazi osalakwa pakati pa dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani kuti likhale cholowa chanu, kuti musakhale ndi mlandu wamagazi. ¹¹ Koma ngati wina amadana ndi mnzake, amamubisalira, namuwukira ndi kumupha mpaka kufa, ndipo akathawira mu umodzi mwa mizindayi, ¹² akulu a mzindawo amutumize kuti akamutenge Kuchokera pamenepo, mum'pereke m'manja mwa wachibale kuti afe. ¹³ Diso lako lisamumvere chisoni; M'malo mwake, ufafanize mlandu wamagazi mu Israeli, kuti zinthu zikuyendere bwino. ¹⁴ Usachotse chizindikiro cha mnansi wako chimene anakhazikitsa kalekale, m inheritancedziko lako limene udzalandire, m thatdziko limene Yehova Mulungu wako akukupatsa kuti ulitenge. ¹⁵ Mboni imodzi yokha sayenera kuwerana ndi munthu chifukwa cha mphulupulu, kapena tchimo lililonse, pa mlandu uliwonse; pakamwa pa mboni ziwiri, kapena pakamwa pa mboni zitatu, nkhani iliyonse iyenera kutsimikiziridwa. ¹⁶ Tinene kuti mboni yosalungama ikauka kutsutsana ndi munthu ali yense kuti acite umboni yakuneneza; ¹⁷ Ndiye kuti onse awiri, omwe akukangana, ayenera kuyimirira pamaso pa Yehova, pamaso pa ansembe ndi oweruza omwe amatumikira masiku amenewo. ¹⁸ Oweruza ayenera kufunsa mwakhama; onani, ngati mboniyo ili mboni yonyenga, ndipo yanenera mbale wake monama, ¹⁹ mum'chitire monga anafuna kuchitira mbale wake; kuti muchotse choipacho pakati panu. ²⁰ Pamenepo otsalawo adzamva ndi kuopa, ndipo kuyambira pamenepo sadzapanganso choipa china chotere pakati panu. ²¹ Maso anu asawamvere chisoni; moyo ulipira moyo, diso kulipa diso, dzino kulipa dzino, dzanja ndi dzanja, phazi ndi phazi.

Chapter 20

¹ Mukapita kukamenyana ndi adani anu, ndipo mukaona akavalo, magaleta, ndi anthu ambiri kukuposa inu, musawaope; pakuti Yehova Mulungu wako ali ndi iwe, amene anakutulutsa m'dziko la Aigupto. ² Pamene mufuna kumenya nkondo, wansembe ayandikire ndi kuyankhula ndi anthu. ³ Awawuze kuti, 'Tamverani Aisraeli, mukumenya nkondo ndi adani anu. Mitima yanu isakomoke. Musaope kapena kunjenjemera. Musaope iwo. ⁴ Pakuti Yehova Mulungu wanu ndiye akupita nanu kukamenyera nkondo pa adani anu ndi kukupulumutsani. ' ⁵ Oyang'anira akuyenera kulankhula ndi anthu kuti, 'Kodi pali munthu wina amene wamanga nyumba yatsopano koma sanayimalize? Amulole abwerere kunyumba kwake, kuti angafe kunkhondo ndipo munthu wina adzipatule. ⁶ Kodi pali munthu amene adalima munda wamphepa koma sadadya zipatso zake? Apite kwawo, kuti angafe kunkhondo ndipo munthu wina asadye zipatso zake. ⁷ Ndi mwamuna uti amene ali pachibwenzi chokwatirana ndi mkazi koma sanamukwatirebe? Apite kunyumba kuti angafe kunkhondo ndipo mwamuna wina amukwatire. ' ⁸ Atsogoleriwo alankhulanso ndi anthuwo nati, 'Kodi pali munthu uti amene wamantha kapena wamantha? Achoke ndipo abwerere kunyumba kwake, kuti mtima wa mchimwene wake usungunuke ngati mtima wake. ' ⁹ Oyang'anira akamaliza kulankhula ndi anthu, awakhazikitse oyang'anira. ¹⁰ Mukapita kukamenyana ndi mzinda, muwapatse mtendere anthuwo. ¹¹ Ngati avomera zomwe akukupatsani ndikakutsegulirani zipata, anthu onse opezeka mmenemo azikhala akapolo anu ndipo akutumikireni. ¹² Koma akapanda kukupatsani mtendere, koma akamenyana nanu, pamenepo muziwuthira nkondo; ¹³ ndipo Yehova Mulungu wanu akakugonjetsani, nawapereka m'manja mwanu, muphe amuna onse a m'mudzimo. ¹⁴ Koma akazi, ana, ziweto, ndi zonse zili mumzinda, ndi zofunkha zake zonse, uzitenge zikhale zako; Mudzatha zofunkha za adani anu, amene Yehova Mulungu wanu wakupatsani. ¹⁵ Muzitero ndi mizinda yonse yakutali kwambiri ndi inu, mizinda yomwe siili mwa mizindayi. ¹⁶ M'mizinda ya anthu awa amene Yehova Mulungu wanu akukupatsani monga cholowa, musasunge chilichonse chopuma. ¹⁷ Mukawawononge kotheratu: Ahiti, Aamori, Akanaani, Aperezi, Ahivi, ndi Ayebusi, monga Yehova Mulungu wanu anakulamulirani. ¹⁸ Chitani izi kuti asakuphunzitseni kuchita chilichonse chonyansa, monga achitira milungu yawo. Mukachita, mudzachimwira Yehova Mulungu wanu. ¹⁹ Mukazungulira mzinda kwa nthawi yayitali, pomenya nawo nkondo kuti muulande, musawononge mitengo yake pomenyetsa nkhwangwa. Popeza ungadye izi, usamaidula. Pakuti kodi mtengo wakuthengo ndi munthu amene muyenera kuzingilira? ²⁰ Mitengo yokha yomwe mukudziwa kuti si mitengo yoti mudyeye, mutha kuwononga ndi kudula; umanga misewu yomenyana ndi mzinda womenyana nawe, mpaka udzagwa.

Chapter 21

¹ Akapezedwa wina wophedwa m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale lanu, ali m'thengo, osadziwika kuti ndani wamuukira; ² pamenepo akulu anu ndi oweruza anu atuluke, ndipo akayese mizinda yoyandikana ndi iye amene waphedwa. ³ Kenako akulu a tawuni yoyandikana ndi mtembo wa mtembowo ayenera kutenga ng'ombe ya ng'ombe yomwe siinayambe yagwirapo ntchito, ndipo sinanyamule goli. ⁴ Kenako azitsogolera ng'ombeyo kupita kuchigwa chokhala ndi madzi, chigwa chomwe sichinalimidwe kapena kufesedwa, ndipo kumeneko ayenera kuthyola khosi la ng'ombeyo. ⁵ Ansembe, ana a Levi, abwere, pakuti Yehova Mulungu wanu anawasankha kuti amtumikire ndi kudalitsa m'dzina la Yehova, ndi kuweruza milandu yonse ya milandu ndi mwano monga mwa mawu awo. ⁶ Akuluakulu onse amzindawo amene ali pafupi kwambiri ndi munthu amene waphedwayo ayenera kusamba m'manja pa ng'ombe yaikaziyo yomwe inathyoka khosi m'chigwa; ⁷ ndipo adzayankha mlanduwu nati, 'Manja athu sanakhetse magazi amenewa, ngakhale maso athu sanawaone. ⁸ Khululuka, Yehova, anthu anu Aisraeli, amene munawaombola, ndipo musakhale ndi mlandu wakupha mwazi wosachimwa pakati pa anthu anu Israyeli. ' Ndiye kukhetsa magazi kukhululukidwa. ⁹ Poto muzichotsa mwazi wosachimwa pakati panu, pamene muchita chokoma pamaso pa Yehova. ¹⁰ Mukapita kukamenyana ndi adani anu ndipo Yehova Mulungu wanu akukupambanitsani ndikuwapereka m'manja mwanu, ndipo muwagwira ngati akapolo, ¹¹ ngati muwona pakati pa ogwidwawo mkazi wokongola, ndipo mumamukhumba mukufuna kumutenga kukhala mkazi wanu, ¹² kenako mudzamutengere kunyumba kwanu; adzameta mutu wake ndikudula misomali. ¹³ Kenako azivula zovala zomwe adavala atagwidwa ndikumakhala mnyumba mwako ndikulirira abambo ake ndi amayi ake mwezi wathunthu. Pambuyo pake uzigona naye ndi kukhala mwamuna wake, ndipo iye adzakhala mkazi wako. ¹⁴ Koma ngati simusangalala naye, ndiye kuti mumulole apite komwe angafune. Koma usamugulitse konse ndi ndalama, ndipo usamuchitire ngati kapolo, chifukwa wamunyazitsa. ¹⁵ Ngati mwamuna ali ndi akazi awiri ndipo m'modzi akonedwa ndipo winayo amadedwa, ndipo onsewo amuberekera ana — onse mkazi wokonedwa ndi mkazi wodana naye — ngati mwana wamwamuna woyamba wa iye amene amamuda, ¹⁶ ndiye tsiku lomwe munthu amapangitsa ana ake kulandira zomwe ali nazo, sangapangitse mwana wa mkazi wokonedwa kukhala woyamba kubadwa asanakhale mkazi wa mkazi amene amamuda, mwana amene ali woyamba kubadwa. ¹⁷ M'malo mwake, ayenera kuvomereza mwana woyamba kubadwa, mwana wa mkazi amene amamuda, pomupatsa magawo awiri pazonse zomwe ali nazo; chifukwa mwana ameneyo ndiye chiyambi cha mphamvu zake; Ufulu woyamba kubadwa ndi wake. ¹⁸ Mwamuna akakhala ndi mwana wamakani ndi wopanduka yemwe samvera mawu a abambo ake kapena amake, ndipo amene, ngakhale atamudzudzula, sadzawamvera; ¹⁹ Pamenepo atate wace ndi amace amugwire, natuluke naye kumka naye kwa akulu a mudzi wace, ndi ku cipata ca mudzi wace. ²⁰ Iwo ayenera kuuza akulu a mzinda wake kuti, 'Mwana wathuyu ndi wamakani ndiponso wopanduka; samvera mawu athu; ndi wosusuka ndi chidakwa. ' ²¹ Pamenepo amuna onse a mumzinda wake azim'ponya miyala kuti afe. kuti muchotse choipacho pakati panu. Aisraeli onse adzamva izi ndi kuchita mantha. ²² Ngati munthu wachita tchimo loyenera imfa ndipo waphedwa, ndipo iwe nkumupachika pamtengo, ²³ ndiye kuti mtembo wake suyenera kugona usiku wonse pamtengowo. M'malo mwake, umuike m'manda tsiku lomwelo; chifukwa aliyense wopachikidwa ndi wotembereredwa ndi Mulungu. Muzimvera lamuloli kuti musadetse dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani kuti likhale cholowa chanu.

Chapter 22

¹ Usayang'ane ng'ombe ya mnzako, kapena nkhosa yake, ikusokera, osabisa; muyenera kuwabwezera kwa iye. ² Ngati mnzako wa ku Israeli sali pafupi ndi iwe, kapena ngati sukumudziwa, uzitenga nyamayo ndi kupita nayo kunyumba kwako, ndipo zizikhala nawe kufikira ataziyang'ana, ndipo um'bwezere nazo. ³ Muchite chimodzimodzi ndi bulu wake; muchite chimodzimodzi ndi chovala chake; inunso muchite naye yense wotayika wa mnzako, yense amene wataya, ndipo iwe wampeza; simuyenera kubisala. ⁴ Usaonenso bulu wa m'bale wako, kapena ng'ombe yake, itagwa panjira, nubisalire; muyenera kumuthandiza kuti ayimikenso. ⁵ Mkazi sayenera kuvala zogwirizana ndi mwamuna, ndipo mwamuna asavale chovala chachikazi; pakuti aliyense wochita izi ndi wonyansa kwa Yehova Mulungu wako. ⁶ Chisa cha mbalame chikakhala patsogolo panu mumsewu, mumtengo uliwonse kapena pansi, muli ana kapena mazira, ndipo mayi atakhala pa ana kapena mazira, musatenge amayi kupita nawo ndi achichepere. ⁷ Uzimasula amake, koma anawo ukhoza kutenga iwe. Mverani lamulo ili kuti zinthu zikuyendereni bwino, ndi kuti mutalike masiku anu. ⁸ Mukamanga nyumba yatsopano, ndiye kuti mupange njerwa padenga lanu kuti musabweretse magazi panyumba yanu ngati wina agwa pamenepo. ⁹ Simuyenera kubzala m'munda wanu wamphesa ndi mitundu iwiri ya mbewu, kuti zokolola zonse zisalandidwe ndi malo opatulika, mbewu zomwe munabzala ndi zokolola za m'munda wamphesa. ¹⁰ Usalime ndi ng'ombe ndi bulu limodzi. ¹¹ Simuyenera kuvala nsalu zopangidwa ndi ubweya wa nkhusa ndi nsalu pamodzi. ¹² Uyenera kudzipangira mphonje pamakona anayi a chovala chimene umadzikongoletsera. ¹³ Tiwerekeze kuti mwamuna watenga mkazi, ndipo napita kwa iye, ndiyeno kudana naye, ¹⁴ ndiyeno kumuneneza za zinthu zochititsa manyazi ndikumuiika mbiri yoyipa, nati, 'Ndinamutenga mkaziyu, koma nditamuyandikira, Sindinapeze umboni wa unamwali mwa iye.' ¹⁵ Kenako bambo ndi mayi a msungwanayo ayenera kupita ndi umboni wokhudza unamwali wake kwa akulu pachipata cha mzindawo. ¹⁶ Abambo a mtsikanayo azinena kwa akulu, 'Ndinampatsa mwana wanga uyu mwamuna kuti akhale mkazi wake, ndipo amadana naye. ¹⁷ Onani, wamuimba mlandu wazinthu zochititsa manyazi nati, "Sindinapeze umboni wa unamwali mwa mwana wako wamkazi." Koma uwu ndi umboni wa unamwali wa mwana wanga wamkazi. ' Akatero, azifalitsa + malayawo pamaso pa akulu a mzindawo. ¹⁸ Akuluakulu a mzindawo amugwire munthuyo ndi kumulanga; ¹⁹ Kenako azimulipiritsa ndalama 100 zasiliva, n'kupereka kwa bambo a mtsikanayo, chifukwa mwamunayo wachititsa mbiri yoipa ya namwali wa ku Israeli. Iye ayenera kukhala mkazi wake; sangamulole kumuchotsa masiku ake onse a moyo. ²⁰ Koma ngati izi zili zowona, kuti chitsimikiziro cha unamwali sichinapezeke mwa mtsikanayo, ²¹ ndiye kuti ayenera kutulutsa msungwanayo pakhomo la nyumba ya abambo ake, ndipo amuna a mumzinda wake amuponye miyala kuti afe, chifukwa mkaziyo wachita chinthu chonyansa mu Israyeli, kuchita uhule m'nyumba ya atate wake; kuti muchotse choipacho pakati panu. ²² Mwamuna akapezeka akugona ndi mkazi amene wakwatiwa ndi mwamuna wina, onse awiri afe, mwamuna amene anagona ndi mkaziyo komanso mkaziyo; kuti muchotse choipacho pakati panu. ²³ Ngati pali mtsikana amene ndi namwali, wotomerana ndi mwamuna, ndipo mwamuna wina amupeza mumzinda ndipo akugona naye, ²⁴ tengani onse awiri kuchipata cha mzindawo, ndipo muwaponye miyala mpaka kufa. Uponye miyala mtsikanayo, chifukwa sanalirire, ngakhale anali mumzinda. Um'ponye miyala munthuyo; chifukwa anaipitsa mkazi wa mnansi wake; kuti muchotse choipacho pakati panu. ²⁵ Koma ngati mwamunayo wapeza mtsikana wolonjezedwa kuthengo, ndipo atamugwira ndi kugona naye, ndiye yekha amene agone nayeyo ayenera kufa. ²⁶ Koma kwa mtsikanayo musamachite chilichonse; palibe tchimo loyenera imfa mwa mtsikanayo. Nkhaniyi ili ngati pamene munthu akumenya mnzake ndi kumupha. ²⁷ Pakuti anamupeza ali kuthengo; mtsikana wolonjezedwa uja analira, koma panalibe womupulumutsa. ²⁸ Mwamuna akapeza mtsikana amene ndi namwali koma sanatomedwe, ndipo atamugwira ndi kugona naye, ndipo ngati apezeka, ²⁹ ndiye kuti mwamuna amene anagona nayeyo ayenera kupereka masekeli 50 a siliva kwa bambo a mtsikanayo, ndipo akhale mkazi wake; Sangamutumize masiku ake onse. ³⁰ Mwamuna asatenge mkazi wa atate wake akhale wake wake; asatengere bambo ake maukwati.

Chapter 23

¹ Palibe munthu amene ziwalo zake zoberekera zaphwanyidwa kapena zodulidwa sangalowe mu msonkhano wa Yehova. ² Palibe mwana wapathengo amene angakhale nawo mumsongkhano wa Yehova; Kufikira mbadwo wakhumi wa mbadwa zake, palibe m'modzi wa iwo akhale m'gulu la Yehova. ³ Muamoni kapena Mmowabu sangakhale mu mpingo wa Yehova; Kufikira mbadwo wakhumi wa mbadwa zake, palibe m'modzi wa iwo akhale m'gulu la Yehova. ⁴ Izi zili choncho chifukwa sanakumane nanu ndi mkate ndi madzi panjira pamene munatuluka mu Igupto, ndiponso chifukwa chakuti anakulemberani Balaamu mwana wa Beori wochokera ku Potori ku Aramu Naharaimu, kuti akutemberereni. ⁵ Koma Yehova Mulungu wanu sanamvera Balaamu; koma Yehova Mulungu wanu anasandutsa tembererolo likhale dalitso lanu, popeza Yehova Mulungu wanu anakukondani. ⁶ Usamafunafuna mtendere kapena mtendere masiku ako onse. ⁷ Usaipidwe naye Mwedomu, chifukwa ndi m'bale wako. usamanyansidwa naye M-aigupto, popeza unali mlendo m'dziko lake. ⁸ Ana obadwa nawo a m'badwo wachitatu atha kukhala a mu mpingo wa Yehova. ⁹ Mukamayenda ngati gulu lankhondo kukamenyana ndi adani anu, mudzisungire kupewa chilichonse choipa. ¹⁰ Ngati pakati panu pali munthu wodetsedwa chifukwa cha zimene zamuchitikira usiku, azituluka mumsasa wa asilikali. asabwerere kumsasa. ¹¹ Madzulo akadzisamba ayenera kusamba; Dzuwa likalowa, azibwerera mumsasa. ¹² Mukhale nawo malo kunja kwa msasa kumene muzikapitako; ¹³ ndipo mudzakhala ndi china mwa zida zanu zokumba nacho; ukadzigwetsa pansi kuti udzipulumutse, uyenera kukumba nayo kenako ndikubwezeretsa nthaka ndikuphimba zomwe zatuluka kwa iwe. ¹⁴ Pakuti Yehova Mulungu wanu akuyenda pakati pa msasa wanu kukupatsani chipambano, ndi kupereka adani anu m'manja mwanu. Chifukwa chake msasa wanu uzikhala wopatulika, kuti angaone chodetsa chilichonse pakati panu ndi kukuchokerani. ¹⁵ Usabweze kwa mbuye wake kapolo amene anathawa kwa mbuye wake. ¹⁶ Akhale nanu pamodzi, m'mudzi uli wonse Iye akasankha. Osamupondereza. ¹⁷ Pasapezeke wachiwerewere wachipembedzo pakati pa ana aakazi a Israeli, kapena pakati pa ana a Israeli. ¹⁸ Usabweretse malipiro a hule kapena malipiro a galu m'nyumba ya Yehova Mulungu wako kuti ukwaniritse lonjezo lililonse. popeza zonsezi zikhale zonyansa kwa Yehova Mulungu wanu. ¹⁹ Usakongoletse Mwisraeli mnzako chiwongola dzanja, chiwongola dzanja cha ndalama, chiwongola dzanja cha chakudya, kapena chiwongola dzanja cha chinthu chilichonse chobweretse chiwongola dzanja. ²⁰ Mlendo ungamubwereke chiwongola dzanja; koma usam'kongoze mnansi wako chiwongoladzanja, kuti Yehova Mulungu wako akudalitse pa zonse udzaikapo dzanja lako, m'dziko lomwe ukupita kulilanda. ²¹ Mukalumbira kwa Yehova Mulungu wanu musachedwe kuikwaniritsa, pakuti Yehova Mulungu wanu adzafuna ndithu kwa inu; kungakhale tchimo ngati inu simukwaniritsa icho. ²² Koma ukapanda kulumbira, sichidzakhala tchimo kwa iwe. ²³ Zomwe zatuluka pakamwa pako uzisunge ndi kuzichita; monga munalumbirira Yehova Mulungu wanu, zonse munazilonjeza ndi mtima wanu wonse; ²⁴ Mukalowa m'munda wamphesa wa mnansi wanu, muzidya mphesa zambiri monga mufuna, koma osataya iliyonse m'dengu lanu. ²⁵ Mukalowa m'munda wa tirigu wakanani wa mnansi wanu, mutha kubudula ngala ndi dzanja lanu, koma osayika chikwakwa cha tirigu kucha wa mnzako.

Chapter 24

¹ Pamenepo Yoswa mwana wa Nuni mwacisinsi anatuma amuna abili kutuluka mu sitimu monga ozonda. Ana kamba, "Yendani, Tanganani paziko, makamaka Teriko." Iwo anayenda na kufika panyumba ya hule wina zina yake anali Rahabi, nakupona mwamwene. ² Zinauziwa kuli mfumu yako yeliko, "ona, bamuna ba ku Israyeli abela kuna kuza zonda (spy) ziko malo." ³ Mfumu yako Jeriko inatuma mau kuli Rahabi na kukamba kuti, "cosa bamuna babwela kuli iwe amene anangena mu nyumba yako, cifukwa ba bwela kuzazonda muziko yonse." ⁴ Koma muzimai anatenga bamuna awili nakuba bisa. Anayankha, "bamuna banabwela kuli ine, koma sini na ziba kwa mene banacoka." ⁵ Banayenda pamene kwenze kofipa, pamene yenze nthawi yovala ciseko ca mu mzinda. Siniziba kwamene bayenda muza bagwira ngati mwaba konka msanga." ⁶ Koma anabakwelesa pamwamba pamalata na kubabisa namitenga yamene anaika pamalata. ⁷ Ndipo bamuna anaba pepeka pa njira yopita ku Yolodani. Ciseko cinavalika pamene opepeka anacoka. ⁸ Bamuna banali basanapone usike, pamene iye anakwela pamalata. ⁹ Anakamba kuti, "niziba kuti Yehova akupasani malo na mantha yoyopa imwe yabwela pali ife. Onse bamene bakhala muziko baza sungunuka pamenso yako." ¹⁰ Tinamvela mwamene Yehova anayumisila manzi ya mu nyanja imwe pamene pamene munacoka ku Egipto. Tinamvelanso vamene munacita kumafumu yabili yaku Amori kumbali ya Yolodani - sihoni na ogi - yamene munabonongelatu. ¹¹ Mwamusanga pamene tinamvela mitima yathu yanasungunuka kunalibe na mphavu inasala muli ali bonse - popeza Yehova mulungu wanu, nimulungu wa mwamba kumwamba na paziko ya pansi. ¹² Manje apa, lumbilani kwa ine zina ya Yehova kuti, mwamene nakhalila nacifundo naimwe, naimwe muzakhalanso nacifundo nanyumba ya batate wanga. Nipaseni cizindikilo ca zooni. ¹³ Kuti muzasunga mayo wa batate banga, bamai binga, abale, alongo banga namabanja yaba yonse, nakuti uzatipulumusa ku imfa." ¹⁴ Bamuna banakamba kuli yeve, "moyo wathu na moyo wanu, ingakuale ku imfa! ngati suzakamba vamene tabwelela, manje pamene Yehova azatipasa malo aya tizakhala nacifundo na ku khulupilika kwa iwe." ¹⁵ Pamene anaba seiusa na nthambo kupitila pa windo. Nyumba mwamene benze kukhala inama ngiwa mulinga ya mumzinda. ¹⁶ Anakamba kwa kuli beve, "yendani kumapili na kubisama olo okonka angakupezeni. Bisamani masiku yatatu paka okonka bakabwelele. Pamene apo yendani ulendo wanu." ¹⁷ Bamuna banakamba kuli yeve, "sitizakhala omangiwa na lonjezu ya lumbilo yamene tinalumbila kuli iwe, Ngati suzacita ici." ¹⁸ Pamene tikabwela muziko, ufunika kumanga nthambo yo fila pawindo pamene watiselusila, na kuika munyumba yako pamozi batate bako na bamai bako ba bale bakona onse ba munyumba ya batate bako. ¹⁹ Alibonse wacoka pa khomo ya nyumba yako kupita munjira, magari yabo yazakhala pamitu yabo ndipo tizakhala tilibe mulandu. koma ngati kwanja kwa ikiwa pali alibonse ali naiwe munyumba, magari yeke yazakhala pamutupako. ²⁰ Koma ukakamba pali ife, tizamasuka kuli lumbilo unatilapisa." ²¹ Rahabi anayankha, "lekani yamene mukamba vicitike." Anababuza bayenda ndipo banayenda pamenepo amanga nthambo yo fila mu windo. ²² Banacoka na kuyenda mumapili nakunkhala kuja masiku yatatu paka okonka bana bwelela. Okonka banasakila munjila yonse koma kulibe camene banapeza. ²³ Bamuna babili banabwelela nakutauka nakubwela kuli Yoswa mwana wa Nuni, na kumu vza vonse vamene vinacitika kuli beve. ²⁴ Bana kamba kuli Yoswa, "Zooni Yehova apasa malo aya kuli ise. Bonse banthu bokhala muziko basungunuka cifukwa chaise."

Chapter 3

¹ Yoswa anauka mumawa, nakutuluka kucoka ku sitimu anabwela ku Yolodani, lye na bana bonse ba Israyeli, ndipo banagona pamene apo basana tauke. ² Pambuyo pamasiku yatatu, basogoleli banapita pakati ka cigono; ³ banalamulila banthu, mukaona likasa ya cipangano ca Yehova mulungu wanu, na ba nsembe ba ku Levi akuinyamula, mufumika kucoka pamalo aya na kuikonka. ⁴ Pafunika kukhala mpata ukulu pakati imwe na yeve yokwanila mikono thu savzande. Osabwela pafupi nayeve, kuti mungaone njiri iti yo yendamo, popeza mukalipe kuyendapo njira iyi." ⁵ Yoswa anakamba nabathu kuti," Zicoseponi mweka mailo, ndaba Yehova azacita vodabwisa pakati panu." ⁶ Ndipo Yoswa anakamba kuli bansembe," nyamujani likasa ya cipangano, na kui pisa pasogolo pabanthu." Iwo ananya mula likasa la cipangano nakuyenda pasogolo yabanthu. ⁷ Yehova anakamba kuli Yoswa kuti," Siku yalelo niza ku kulisa mumenso ya Israyeli yonse. Bazaziba kuti mwamene nenzeli na Mose, nizakhalansu naiwe. ⁸ Uzalamulila bansembe bamene banyamula likasa la cipangano,' pamene wafika posilizila mazi ya Yolodani, Ufunika kulimilila mu mana wa Yolodani." ⁹ Ndipo Yoswa anakamba kuli bana ba Israyeli, " bwelani kuno, na kumvela mau ya Yehova mulungu wanu. ¹⁰ Pali ici muzaziba kuti mulungu wa moya ali pakati panu na kuti azapisha pamensopanu Akanani, na Ahiti, na Ahivi, na Apeiezi, na Agiligasi, na Amoli, na Ayebusi. ¹¹ Onani! Likasa ya cipangano ca Ambuye waziko yonse yapansi itauka pasogolo pano mu Yolodani. ¹² Manje bamuna ba twebu bocoka kumitundo ya Israyeli, mwamuna umozi kucoka kumutundu umozi. ¹³ Pamene mapazi ya bansembe bamene banyamula likasa ya Yehova, Ambuye wa ziko yonse, gwila manzi ya mu Yolodani, manzi ya mu Yolodani yazaduliwa, namanzi yamene yayendela pansi kucokela mumumana wapa mwamba ya zaleka kuyenda yazaimilila pamozi. ¹⁴ Pamene banthu banacoka kutauka pa Yolodani, wansomba amene ananyamula likasa ya cipangano anayenda pasogolo ya banthu. ¹⁵ Mwamsanga pamene baja banali kunyamula likasa bana fika pa Yolodani, namapaja yabaja bananyamula likasa ya ikiwa mu mbali yamazi (manje Yolodani ataikila mumbali zonse, nthaw! yokolola), ¹⁶ manzi yamene yanataikila kucoka pamumana wapamwa mba yanaimilila pamozi. Manzi yanaleka kutaikila kucokela kutali. Manzi yanaleka kutaikila kucoka ku Adamu, muzinda uli pambali ya Zarethani, kuyenda pansi kunyanja ya Araban, nyanja ya mucele. Banthu banatauka pafupi na Yeriko. ¹⁷ Bansembe bamene bananyamula likasa ya cipangano ca Yehova banaimilila pamalo yoyuma mukati miva Yolodani paka banthu bonse ba Israyeli banatauka panthaka yoyuma.

Chapter 4

¹ Pamene banthu onse banatauka pa Yolodani, Yehova anakamba kuli Yoswa, ² "Sankhani bamuna bali twevu kucoka pakati kabanthu, munthu umozi kucoka kumutundu umozi. ³ Bapase lamulo: tengani miyala yali twevu kucoka pakati ka Yolodani pamene bansembebai milila pamalo yoyuma, na kuyaleta na kuyafaka panso malo mwamene muzagona usiku walelo. ⁴ Ndipo Yoswa anaitana bamuna twevu bamene anasankha kucoka kumitundo ya Israyeli, umozi kucoka kumutundu ulibonse. Yoswa anakamba kuli beve, "Yendani kusogolela likasa ya Yehova mulungu wanu pakati pa Yolodani. ⁵ Alibonse waimwe afanika kunyamula mwala paphewa, kulinga na nambala ya mitundu ya bana ba Israyeli. ⁶ Ici ndiye cizakhala cizindikilo canu pakati panu pamene banu bazafunsa masiku yamene yabwela, 'Aya miyala yatanthauza canu kuli imwe?' ⁷ Pamenepo muzakamba kuli beve, 'manzi ya Yolodani yanaduliwa pasogolo palikasa ya cipangano ya Yehova. Pamene inatauka pa Yolodani, manzi ya mu Yolodani yanaduliwa cifukwa chake aya miyala yazakhala yokumbukilapo kubana ba Israeli muyaya.'" ⁸ Bana ba Israyeli banacita mwamene Yoswa analamulila, ndipo ananyamula miyala ili twevu pakati ka Yolodani, mwamene Yehova anakambila kuli Yoswa. banafaka miyala kulingana nanambala yamitundu ya bana ba Israyeli. Bana nyamula miyala kwalu kwamene balagona na kuyafaka kwamene. ⁹ Pamenepo Yoswa anafaka miyala yali twevu pakati ka mumana wa Yolodani, mumalo mwamene mapazi ya bansembe bananyamula likasa yacipangano banaimilila. Cokumbukilapo cilipo nalelo. ¹⁰ Bansense bananyamula likasa banaimilila pakati pa Yolodani paka vonse vame Yehova analamulila Yoswa kubuza banthu vinasila, kuli ngana navamene Mose analamulila Yoswa. Banthu banayendesa nakutauka. ¹¹ Pamene banthu banasiliza kutauka, likasa ya Yehova ina tauka pamenso ya banthu. ¹² Mutundu wa Rubeni, mutundu wa Gadi, na mutundu wa pakati wa manase unatauka pamenso ya bana ba Israyeli na kupanga gulu yankhundo, monga mwamene Mose anakambila kuil beve. ¹³ Bamuna okwanila fote sauzandi okonzela nkundu banatauka pamenso ya Yehova, ku nkundu ku zidikha za Yeliko. ¹⁴ Pasiku ija Yehova anakulisa Yoswa mu mensu ya Israyeli yonse. Banamulemekeza mwamwene bana lemekezela Mose - masiku yake yonse. ¹⁵ Ndipo Yehova anakamba kuli Yoswa, ¹⁶ "Lamulila wansembe wamene anyamula likasa ya umboni kuli acoke mu Yolodani." ¹⁷ Pamenepo, Yoswa analamulila ba nsembe," cokani muni mu Yolodani." ¹⁸ Pamene bansembe bonyamula likasa ya cipangano ca Yehova banacoka pakati pa Yolodani namapazi yabo yananyamuliwa kucoka pamalo yoyuma, manzi ya Yolodani yanabwelela ku malo yake nakutauka magombe, monga mwamene yanalili masiku fo (4) yapambuyo. ¹⁹ Banthu banatuluka kucoka mu Yolodani pasiku ya numbala teni mu mwezi woyamba, Bana khala mu Giligo, kumawa kwa Yeliko. ²⁰ Miyala ili twevu yamene bana nga mu Yolodani, Yoswa anayafaka mu Giligo. ²¹ Anakamba kubana ba Israyeli, "pamene bana bafunsa batate babo masiku yobwela, 'Aya miyala niya canu?' ²² Babuzeni bana, 'Apa niye pamene Israyeli ana taukila pa dothi yuyuma.' ²³ Yehova mulungu wanu anayumisa manzi ya mu Yolodani, paka munatauka, monga mwa Yehova mulungu wanu anacitila kunganja Yofila, yamene ana yumisa paka tinatauka, ²⁴ kuti banthu bonse banucalo bazibe kuti zanja ya Yehova niya mphamvu, nakuti muzalemekeza Yehova mulungu wanu muyayaya.

Chapter 5

¹ Mwamusanga pamene mafumu ya Amori kumbali ya kumazulo kwa Yolodani, na mafumu yonse ya Akanarli, bamene banali mumbali mwanya nja yaikulu, banamvela kuti Yehova anayumisa manzi ya mu Yolodani paka bana ba Israyeli anatauka, mitima yao yanasungunuka, ndiponso munalibe moyo anasalamo muli beve cifukwa ca bana ba Isreali. ² Panthawi Yehova anakamba kuli Yoswa, "panga manaifi ya miyala na kujuba bonse bana ba Israyeli kacibili." ³ Pamenepo Yoswa anapanga manaifi yamiyala nakujuba bonse bana ba Israyeli pa Gibeath, Haaraloth. ⁴ Ndiye cifukwa cake Yoswa anaba juba: Bonse bamuna bamene banacoka mu Eigipito, kufakilako nabazibambo bankhondo, anafa mucipululu munjila, pambuyo pacokokamu Eigipito. ⁵ Ingakuale bamuna bonse banacoka mu Eigipito banali bujubiwa, cimizi-mozi, palibe anyamata bana wila mucipululu munjila yocoka ku Eigipito anajubiwa. ⁶ Pakuti bana ba Israyeli banacoka zaka fote mu cipululu paka bathu bonse, niye, bonse bazibambo bankhondo banacoka mu Eigipito, anafa, cifukwa sanamvelela mav ya Yehova. Yehova analumbila kwaiwu kuti sazabasiya kuti babone malu yamene analumbila kuli makolo yao kuti azabapasa, ziko yoyendemo mkakana uchi. ⁷ Banali bana bao bamene Yehova anakulisa mumalo yao bamene Yoswa anajuba, cifukwa banali bakalibe kujubiwa munjira. ⁸ Pamene onse bana jubiwa, banasalila kwamene banali kugona paka bana pola. ⁹ Ndipo Yehova anakamba kuli Yoswa, "Siku yalelo na cosapo manyazi ya Eigipito pali imwe, cifukwa chake, zina ya malo inaitaniwa Giligala kufika nalelo. ¹⁰ Bana ba Isreali banamanga misasa pa Giligala. Basunga paka pasiku ya fotini ya mwezi, mu mazulo, madimba ya yaliko. ¹¹ Pasiku ya paska, siku yamene ija, bana dya vina vomela pa nthaka, mkate wopanda cotuposa na tiligu wokazinga. ¹² Mana yanasiya pasiku banadya vomela pathaka. Kunaliba futi mana ya bana ba Israyeli, koma banadya vomelapanthaka ya kanani caka cija. ¹³ Pamene Yoswa anali pafupi na Yeliko, ananyamula mwenso yake na kuona, ndipo taona, mwamuna anaimilila pasogolo pake; anatenga panga nipo inali mumanja yake. Yoswa anayenda kuli yeva na ku kamba kuti, "Uli naise kapene badani bathu? ¹⁴ Anakamba kuti," lyai. Popeza ndine bolamulila gulu ya nkhondo ya Yehova. Manje nabela." Pamenepo Yoswa anagwesa nkhope yake pansi kulambila nakukamba kuli yeve kuti, "Akamba cani Ambuye wanga kuli mtumiki wake?" ¹⁵ Bolamulila gulu ya nkhondo ya Yehova anakamba kuli Yoswa, "vula nsapato zako ku mapazi yako cifukwa pamalo pamene waimilila ni poyela," ndiye zimene Yoswa anacita.

Chapter 6

¹ Manje ponse pongenela ku Yeliko panavaiwa cifukwa ca gulu ya nkondo ya Israyel. Kulibe anacoka olo kungena. ² Yehova anakamba kuli, "ona, napasa Yeliko mu manja yako, mfumu yao, na ba silikali ba phunzila. ³ Ufunika kuzunguluka muzinda, bonse bamuna bankhondo kuzunguluka mzinda kamozi. mufunika kucita ici masiku zikisi. ⁴ Bansembe bali seveni bafunika kungamula malupenga ya bana ba nkhoa zamasengo pasogolo ya likasa. Pasiku ya seveni, ufunika kuzunguluka muzinda kali seveni, na bansembe bafunika kuliza mphalaza pamalupenga. ⁵ Pamenepo bafunika kuliza mpalasa yitali na masengo ya mwana wankhosa, mukamvela kulila kwa lupenga bantu bonse bafunika kupunda maningi, na cipupa ca muzinda cizangwa pansi. Basilikali bafunika kumenya alibonse kuyenda kwake." ⁶ Ndipo Yoswa mwana wa Nuni anaitana ba nsembe na kukamba kuli beve," nyamula likasa ya cipangano, leka bansembe bali seveni banyamule malupenga yali seveni ya nkhoa masengo kusogolo kwa likasa ya Yehova. ⁷ Anakamba kuli banthu, "Yendani mukazunguluke muzinda, na bamuna bankhondo bazayenda pasogolo pa likasa ya Yehova. ⁸ Monga mwamene Yoswa anakambila kuli banthu, bansembe bali seveni bananyamula malipenga yali seveni ya nkhoa, masengo pamenso ya Yehova. Pamene banayenda pasogolo, banaliza mphala pa lupenga. likasa ya cipanga ca Yehova ina konkapo pambuyo pabo. ⁹ Bamunabokonzeka bankhondo banayenda pasogolo pa ba nsembe, nipo banaliza mphalasa pa malupenga, koma olonda banabwela mumbuyo mwa likasa, na bansembe banaliza malupenga mopitiliza. ¹⁰ Koma Yoswa analamulila banthu, kukamba kuli, "Osakuwa. pakanwa panu pasacoke mav paka siku nizaazani kukuwa. pamenepo mufunika kukuwa." ¹¹ Tele analengesa likasa ya Yehova kuzunguluka muzinda kamozi siku ija. Ndipo banaluba mucipono cabo, na kukhalamo usiku mucigono. ¹² Ndipo Yoswa anauka mumawa, na bansembe banatenga likasa ya Yehova. ¹³ Bansembe bali seveni, bamone benze kunyamula malupenga yali seveni yankhosa' masengo kusogolo kwa likasa ya Yehova, banayenda bwino nakuliza mphalasa pa malupenga. Basilikali akonzeka banali kuyenda pasogolo pabo. Koma pamene olonda banayenda pasogolo pa likasa ya Yehova, malipenga ayanpeleka kulila kopitiza. ¹⁴ Banazunguluka muzinda kamozi siku lacibili na kubwela ku cigano. Banacita ivi masiku sikisi. ¹⁵ Panali pasiku ya namba seveni pamene banauka mumawa, banazunguluka muzinda munjila imozi mwamene banali kucitila, iyi nthawi kali seveni, panali pasiku ya kuti anazunguluka kali seveni. ¹⁶ Panali pasiku ya seveni, pamene uba nsembe banaliza mphalasa na malupenga, kuti Yoswa analamulila bantu, "kuwani" popeza Yehova akupasani muzinda. ¹⁷ Muzinda navonse vilimo vizapatuliwa kuli Yehova kuvi bononga, Rahabe hule chabe ndiye azakhala - yeve nalonse bamunyumba yake - cifukwa anabisa ba muna tinatuma. ¹⁸ Koma kuli imwe yanganani pavinthu vopatuuliwa kuonongewa, kuti muvi conge kuti vinengewe, sumuzatengapo cili conse. mukacita izo, muzapanga cigono ca Israyeli cinthu cina camene cifunika kuonongewa ndipo nuza bwelesa mavuto. ¹⁹ Siliva yonse, Golide, navinthu vopangiwa na bronzi na nsimbi vapatuliwa kuli Yehova. Vifunika kulowa mu chuma cha Yehova. ²⁰ Pamene banaliza mphalasa na malupenga, bantu banapunda maningi navipupa vinagwa pansi. Ndipo mwa muna aliyense anayenda mukati nakutenga muzinda. ²¹ Banaongelatu vonse mumzinda nalupanga - mwamuna na mkazi, mingono na mkulu, ng' mbe, nkhoa na abulu. ²² Ndipo Yoswa anakamba kuli bamuna babili bamene banaona malo, "Yendani muyumba ya hule. Cosani muzimai navonse vili munyumba mwake, mwamene munalumbilila kuli yeve. ²³ Pamenep bamuna bacicepele bamene banali bobona banangena nakucosa Rahabi. Banaacosa batate bake, bamai bake, ba bale bake, na ba bale bake bonse bamene benze nayeve. Anabaleta pamalo yali kunju kwa Israeli. ²⁴ Bana shoka muzinda na vonse vili mukai. Ni siliva, Golide, na vida va Bronzi vinafakiwa mucuma ca munyumba ya Yehova. ²⁵ Koma Yoswa anavomekeza Rahabi hule, banja ya batate bake, na vonse venze nayeve kunkhala. Akhala mu Israyeli lelo cifukwa anabisa bamuna bamene Yoswa anatuma kubona Yeliko. ²⁶ Ndipo Yoswa anabalamulila ija nthawi na kulumbila, anakamba kuti, "Wotembeleleka ni muntu mu menso ya Yehova wamene amanga muzinda wa Yeliko, pakupeleka mwana woyamba azamanga maziko, pakupeleka mwana mung'ono, uzapanga viseko. ²⁷ Ndipo Yehova anani na Yoswa, na mbili yake inayenda muziko yonse.

Chapter 7

¹ Koma bana ba Israyeli banacita mosakhulupilika pavi nthu vamene vina patuliwa kuti vionengewa. Achani mwana wa Karmi mwana wa Zabdi mwana wa Zerah, kucokela kumtundu wa Ayuda, anatenga vinthu vina vamene vinapatuliwa kuti viongeke, nakukalipa kwa Yehova kunayakila pali bana ba Israyeli. ² Yoswa anatuma bamuna kucoka ku Yeliko kupita ku Ai, yamene yenze pafupi na Beth Aven, kumawa kwa Bethel. Anakamba kuli beve, yendani na kukauna ziko." Bamuna baja banayenda na kuona Ai. ³ Pamene bana bwelela kuli Yoswa, banakamba kuli yeve osatuma bantu bonse ku Ai. Tumani cabe bamuna bali twu sauzande olo fili sauzande kuyenda kumenya Ai. Osalengesa bantu onse ba sebenze munkhondo cifukwa ni bang'ono." ⁴ Potelo bamuna cabe bali fili (3) sauzande ndiye banayenda kucoka pali basilikali, koma banathaba aba kuli bamuna baku Ai. ⁵ Bamuna ba ku Ai banapaya bamuna ba feti sikisi pa mene anaba pepeka kucokela pakhomu yamuzinda kufika kumalo yamiyala, nakubapaya pamene benze kuyenda pansi pa phiri. Mitima ya bantu yana sungunuka nonkhala monga mansi. ⁶ Ndipo Yoswa anang'amba vovala vake. Yeve na bakulu ba mu Israeli banaika dothi pamitu yao na kugwesa nkhope zao pansi pasogolo ya likasa ya Yehova, kunkhala paja paka usiku. ⁷ Ndipo Yoswa anakamba kuti, "Ha, Yehova Ambuye, cifukwa cani mwavomekeza aba banthu pufika pa Yolodani? Kutipasa mumanja ya Amoni kuti bononga ise? Ngati cabe tinapanga maganizo yosiyana nakunkhala kumbali ina ya Yolodani!" ⁸ Ambuye, ningakambe cani, popeza Israyeli abwelela mumbuyo pamenso yandani bake? ⁹ popeza Akanani nabonse bokhala muziko baza mvela ici. Bazati zunguluka nakupanga banthu ba paziko kuibala zina yathu. muzaeita cani pa zina yanu ikulu? ¹⁰ Yehova anakamba kuli Yoswa, "nyamuka! nicanu wagwesela nkhope yako?" ¹¹ Israyeli wacimwa. Banaphwanya cipangano canga camene nina balamulila. Aba vinthu vina vamenevi napatuliwa. Aba nakubisa macimo yabo pakuika vameneba pakati ka vinthu vabo. ¹² Cifukwa caici, bana ba Israeli sibanga imilile pali badani bao. Banabwelela mbuyo kuthaba badani bao cifukwa beve bapatutuwa kuti ba bonongeka. Sinazakhala futi naimwe pokhapo muononge vinthu venze kufunika kubongewa, koma vikali pakati kaimwe. ¹³ Nyamukani! patulani banthu kwaine na kukamba nabo kuti, zipatuleni mweka kukonzekela mailo, popeza Yehova, mulungu wa Israeli "akamba kuti," kuli vinthu vopatuliwa vofunika kubongewa vili pakati kaimwe Israyeli simunga imilile pali badani bani paka mucose pakati kanu vinthu vonse vamene vinapatuliwa kubungewa. ¹⁴ Mumawa, mufunika kuzionesa kulingana namutundu wano. mtundu wamene Yehova asankha uzabwele pafupi na abale bao. Mfuko yamene Yehova wasankha ifunika kufika pafupi naba munyumba. Bamunyumba bamene Yehova asankha bafunika kubwela umozi omozi. ¹⁵ zizacitika kuti wamene asankhiwa na wamene ali na vinthu vina patuliwa kuti vibongewe, Aza shokewa, yeve navonse alinavo, cifukwa aphwanya cipangano ca Yehova na cifukwa acita cintu comvesa manyazi mu Israyeli." ¹⁶ Ndipo Yoswa anabuka mumawa nakuleta Israyeli pafupi, mutundu na mutundu wa Ayuda unasankhiwa. ¹⁷ Yoswa analeta mafuko ya Ayuda pafupi, na mfuko ya Zerahites inasankhiwa. Analeta pafupi mfuko ya Zerahites munthu na munthu, na Zabdai anasankhiwa. ¹⁸ Analeta bamunyumba ya Zabdi pafupi, munthu na munthu, na Achani mwana wa Karmi, mwana wa Zabdi, kucoka kumutundu wa Ayuda, anasankhiwa. ¹⁹ Pamenepo Yoswa anakamba kuli Achari, "mwana wanga, kamba cazoona pamenso ya Yehova, mulungu wa Israeli, na kupeleka zokamba zako kwa yeve. Nibuze camene wacita, osanibisa ine." ²⁰ Akani anayankha Yoswa, "zoona, naci mwila Yehova, mulungu wa Israyeli. Izi niye zamene ninacita: ²¹ Pamene nina bona pakati ka votengewa covala cokongola ca ku Babiloni, masikelo yali thu handiledi ya siliva, na cikute ca golide kelemela masikelo fifite, ninavi khumbwa nakuvitenga. Nivobisiwa pansi pakati ka cihema, na siliva ili pansi pake." ²² Yoswa anatuma amithenga, banathamangila kuhema na kuja kunali vinthu. Pamene bana yang'ana, bana vipeza nivobisiwa mu hema yake, na siliva pansi pake. ²³ Banate vinthu kucoka pakati ya hema na kuvileta kuli Yoswa nakuli bonse bana ba Israyeli. Banavitula pamenso ya Yehova. ²⁴ Ndipo Yoswa, na Israyeli onse na yeve, Banatenga Achani mwana wa Zerah, na siliva, na covala, acocikule ca golide, bana bake bamuna na bakazi, ng'ombe zake, mabulu, mkhosa, na heme yake na vonse enze navo, nipo banavileta kucigwa ca Achor. ²⁵ Pamenepo Yoswa anati, nicanu camene wativutula? Yehova azakuvuta lelo." Bonse ba Israyeli ba mutema na miyala. Na bonse bosalila ba natemewa namiyala naku shokewa na mulilo. ²⁶ Bana mukila miyala yambili pamozi kufika nalelo. Yehova anacosapo ku kwiya kwake. cifukwa cake zina ya malo ni cigwa ca Achor paka kufika nalelo.

Chapter 8

¹ Yehova anakamba kwa Israyeli." Osayopa; osabwelela mumbuyo. Tenga bantu bonse bankhondo. Yenda ku Ai, nakupasa mumanja mwako mfumu ya ku ai, bantu bake, muzinda wake, na malo yake. ² Vzacita kuli A na mfumu zake monga mwamene unacitila ku Yeliko na mafumu yake, koma votengwa na vobeta uzatenga. Vyike bantu kumbuyo kwa muzindi." ³ Ndipo Yoswa ananyamuka nakutenga bamuna bonse ku Ai, pamene apo Yoswa anasankha bamuna bali feti sauzande - okosa, bamuna ba mphavu - anabatuma kuyenda busiku. ⁴ Anabalamulila, "onani, muzagonela kumbuyo kwa muzinda, osayenda kutali kucoka mu muzinda, koma monse imwe konzekani. ⁵ Ine nabamuna bonse bali naine tizafika ku mzinda, pamene ibo bakacoka ku menya ise, tizathaba kuli beve mongo tinacitila poyamba. ⁶ Bazacoka kutikonka paka tibacose ku muzinda. Bazakamba kuti, bali kuti thaba monga mwamene banathambila! naise tizabathaba. ⁷ Pamenepo muzacoka malo mwamene munabisama, nakulowa mumzinda. Yehova mulungu wanu azakupasani mumanja yanu. ⁸ Pamene mwagwila muzinda, muza ushoka, muzacita ivi pamene mwamvelela cilamulo capasiwa mumav ya Yehova ona, nakulamulila." ⁹ Yoswa anabatuma, banapita kumalo yabiamamo, na kubisama pakati ka Beteli na Ai ku mazulo ya Ai. koma usiku uja Yoswa anagona pakati ka banthu. ¹⁰ Yoswa anabuka kuseni maningi na ku konzekela basilikali bake, Yoswa na bakulu ba Israyeli, na kumenya bathu baku Ai. ¹¹ Bamuna bonse bankhonda bamene banali naye banayenda kufika mumzinda. Banafia pafupi namuzinda nakumanga misasa kumbali yaku mpoto kwa Ai, Manje panali cigwa pakati pao na Ai. ¹² Anatenga bamuna a Faivi (5) sazande na kui ka mobisika kumbali ya ku mazulo kwa muzinda pakati ka Beteli na Ai. ¹³ banaimika ba silikali bonse, gulu ya nkondo ikulu kumpoto kumbali kwa muzinda, na olonda kumbali yakumazulo kwa mzinda. Yoswa anagona mucigwa usiku uja. ¹⁴ Zinacita pamene mfumu ya ku Ai inacibona, na gulu yake yankhondo inauka kuseni nakucoka kuyenda kumenya Israyeli pamalo pena yamene kuthila mucigwa ca mumana wa Yolodani, sanazibe kuti baja bobisama banali kuyembekeza kumenyela kumbuyo kwa muzinda. ¹⁵ Yoswa na Israyeli bonse banalekelela kuti bagonjesewe pamenso pao, na kuthabila ku cipululi. ¹⁶ Onse bantu banali mu mzinda banaitaniwa kuti ba pepeke, ndipo banapepeka Yoswa nakucosewako ku muzinda. ¹⁷ Kulibe munthu alibonse anasalila mu Ai na Beteli amene anayenda kupepeka Israyeli. Banasiya muzi kopanda aliyense pamene banapepeka Israyeli. ¹⁸ Yehova anakamba kuli Yoswa, "penyesa mkondo uyo uli mumanja yako ku, popeza nizapasa Ai mumanja mwako." Yoswa anacosa mukundo unali manja mwake kupenyesa ku muzinda. ¹⁹ Basilikali bobisama msanga banathmanga kucoka mumalo yao pamene anatambasula kwa nja kwake. Banathamanga nakungena mumuzi na kuutenga. mwamsanga bana shoka muzi. ²⁰ Bamuna baku Ai banapindamuka hakuyangana ku mbuyo. Banabona cusi kucoka mumzinda ciyenda mumwamba, pamenepo banakanga kuthabila ukukapena uko. popeza basilikali ba Israyeli bamene banathabila mucipululu manje banabwelela kukumana nabaja benza kuba pepeka. ²¹ Pamene Yoswa na Israyeli banaona kuti bobisama banatenga muzinda na cusi ciyenda mwamba banabwelela nakupaya bamuna ba ku Ai. ²² Bena banatuluka mumuzinda kuba menya, kuti ibo banagwiliwa pakati, na Israyeli pakati, bena kumbali na mbali ija. Israyeli anameya bamuna baku Ai palibe anapuluma kapeka kuthaba. ²³ Banasunga mfumu ya ku Ai, wamene banagwira wamoya na ku muleta kuli Yoswa. ²⁴ Pamene Israyeli anasiliza kupaya bonse bokhala mu Ai mumunda pifupi nacipululu kwamene anaba pepeke, napamene bonse, kufikila wosilizila, anagwa na lupanga Israyeli bonse anabwelela ku Ai, Banamenya Ai na lupanga. ²⁵ Bonse banagwa siku ija, bonse bamuna na bakazi, benze tyovu sauzandi (12), bonse banthu ba mv Ai. ²⁶ Yoswa sanabweze kwanja kwake kwamene anatambasula pamene anagwila mukondo, paka anabonongelatu banthu bonse ba mu Ai ²⁷ Israyeli anatenga vobeta navtenga kucoka mumzinda, monga mwamene Yehova anabalamulila Yoswa. ²⁸ Yoswa anashoka Ai na kuusandusa muunda wamavuto muyaya. Nimalo yosiyiwa kufika lelo ²⁹ Anapaci, a mfumu yaku Ai pamtengo paka mazulo. Pamene zuba yenze kungena, Yoswa anapa lamulo na kuseluse thupi yamfumu nakuika pasogolo pakhomu ya muzinda. pamenepo banaikapo miyala ikulu ya mbiri pamwamba pake. Yaja miyala yalipo kufika lelo. ³⁰ Pamene Yoswa anamangila Yehova gowa, mulungu wa Israyeli, pa pili ya Ebal, ³¹ Monga mwamene Mose mutumiki wa Yehova analamulila bana ba Israyeli, mwamene cinalembewela mubuku yacilamulo ca Mose." Guwa kucoka kumiyala yosajubiwa, pamene kulibe anapangilapo cisulo cansimbu," Anapeleka nsembe zo pseleza paguwa kuli Yehova, nakupeleka nsembe zamtendele. ³² Pamenepo mumenso ya bana ba Israyeli, malemba pamiyala cisanzo calamulo ya mose. ³³ Israyeli bonse, bakulu bao, bobayang'anila, na boweliza banaimilila kumbali zonse zibili zalikasa pamenso ya bansembe na Alevi bananyamula likasa yacipangano ca Yehova - mlendo na bobadwila muziko bena pali beve banaimilila kusogolo kwa phili ya Gelezimu na bena kusogolo kwa phili ya Ebal. Bana ba Israyeli, monga mwamene Mose mtumiki a mulungu anabalamulila poyamba. ³⁴ Pambuyo pake, Yoswa anabelenga mau yonse ya cilamulo, madaliso na matembelelo, monga mwamene banayalembela mubuku ya lamulo. ³⁵ Kunalibe mau yalilyonse yamozi kuli vonse Mose

malamulila vamene yoswa sanabelenge kusogolo kwa gulu ya Israyeli, kufakilako bazimai, bana bang'ono nabalendo banakhala pakati pao.

Chapter 9

¹ Ndipo mafumu yonse yanakhala kusogolo kwa Yolodani muziko ya mapili, na malo ya pansi ya munyanja kufupi na Lebanon - mu Hittites, Amoni, Akanani, Aperizzites, Hivites, na ajebusites - ² Zonse zina lumikizanz pansi pa lamulo imozi, kuchaya nkondo na Yoswa na Israyeli. ³ Pamene bonkhala mu Gbeoni banamva vameneyoswa anacita kuyeliko na ku Ai, ⁴ Banapanga mapiani mocenjeia, Banayenda monga amithenga Banatenga masaka yong'ambika nakuyafakaa pa mabulu banatenganso vikumba va vinyu wakudala vong'ambika, ndipo vinakonzewa. ⁵ Bavala nsapato zakale na zongambika kumapazi yao, nakuvala vakale, vovala vong'ambika, mikate yonse muumalo yosungilamo inali yoyuma. ⁶ Ndipo banayenda kuli Yoswa mucipono ca Giligala nakukamba naye naba muna ba mu Israyeli, "tacokela kuziko yakutali, Apa manje panga cipangano naise." ⁷ Bamuna bamo Israyeli banakamba kuli ba Hivites, "kapena munkhala pafupi naise. Tingapange bwanji cipangano naimwe?" ⁸ Banamba kuli Yoswa kuti, "Ise ndise batumiki bano." Yoswa anakamba na beve, "Ndiwe ndini? munacokele kuti?" ⁹ banakamba kuli iye, "Batumitiki bako babwela kuno kucokela kumalo yakutali, cifukwa ca zina ya Yehova mulungu wanu. Tamvela pali yeve na pali vonse anacita mu Eipito - ¹⁰ navonse anacita kuli mafumu yabili yako Amoni kumbali ina ya Yolodani - kuli sihon mfumu ya Heshbon, na ku og mfumu ya Bashan amene enze pa Ashtaota. ¹¹ Bakulu banthu na bonse bonkhala muziko banakamba naife, nyamulani vokudya muulendo wanu. Yenda kukumana nabeve na kukamba nabo," ndife batumiki banu pangana ni nafe," ¹² Uyu ndife mkate wanu, vnali ukuli wakupsa pamene tina utenga kucosa manyumba yathu pasiku tinacoka kubwela kuli imwe koma manje, ona, niyo yuma na kuzizila. ¹³ Ivi vikumba va vinyu vakale vinali va nyowani pamene tinavi zuza manje ona, manje vinang'ambika vovala vathu na nsapato zathu zasilila ku olendo utali ¹⁴ Pamenepo ba Israyeli banatenga vokudya vina, koma sanafunse Yehova kubabuza vocita. ¹⁵ Yoswa anapanga mutendele na beve na kupanga cipangano nabeve, kubasiya na moyo. Basogoleli babanthu nabeve banalumbilila kuli beve. ¹⁶ Masiku yatatu bana ba Israyeli atapanga cipangano na beve, banamvela kuti banali kukhala nabo pafupi. ¹⁷ Ndipo bana ba Israyeli banayambapo nakufika kumizinda yao pasiku yacitatu. mizinda yao yanali Gibeoni, Kephirah, Beeroth, na Kiriath Jearim. ¹⁸ Bana ba Israyeli sanabamenye cifukwa basogoleli bao banalumbulila pali beve pamenso ya Yehova, mulungu wa Israyeli, Ba Israyeli bonse banali kudandavla pali asogoleli bao. ¹⁹ koma basogoleli bonse banakamba kuli banthu bonse," tina ba lumbililako kwa Yehova, mulungu wa Israyeli, manje sitinga bacite. ²⁰ Izi ndiye tizacita kuli beve: kupewa ukali wamene ungabwele pali ise cifukwa ca lumbilo yamene tinalapa kuli beve." ²¹ Basogoleli banakamba kuli banthu bao, "nkhalala na moyo." ndipo ba Gibeonites banakhala wojuba maplanga na botapa mazi ya bana ba Israyeli, monga mwamee ba sogoleli anakambila pali beve. ²² Yoswa anabaitana na kukamba kuti, "cifukwa nicani ananinama pamene unakamba, tili kutali naimwe, pamene ukhala pakati kaise?" ²³ Manje, cifukwa caici, ndiwe otembeleleka nabena baimwe muzayamba kukhala akapolo, naja wodula maplanga na botapa manzi ya nyuma ya mulungu." ²⁴ Banayankha Yoswa na kukamba kuti, "cifukwa cinauziwa kuli batumiki kuti Yehova mulungu analamulila mtumiki wake Mose kukupasani malo yonse, nakubononga bonse bokhala mumalo pamenso yanu - ndipo ticitila miyoyo yathu mantha cifukwa ca ino. Cifukwa cake tinacita cinthu ici cinthu. ²⁵ Manje, ona, utigwila mu mphamvu yako. ciliconse coboneka cabwino na colungama kucitila ife, cita." ²⁶ Potelo Yoswa anabacitila ici: Anabacosamo muulamulilo wa bana ba Israyeli, kuti Israeli basaba paye. ²⁷ Siku yame Yoswa anakumana nabo juba maplanga ma Gibeonites na botapa manzi mu muzi, na paguwa ya Yehova, paka lelo, mumalo yamene Yehova anasankha.

Chapter 10

¹ Manje pamene Adoni - Zedeki, mfumu yaku Yelusalemu, inamva kuti Yoswa anatenga Ai nakuionongelatu (monga mwamene banacitilaku Yeliko na mfumu yake), anamvelanso mwamene bantu ba ku Gebeoni banapangila mtendele na Israyeli nakunkhala pakati kao. ² Bana ba Israyeli banayopa maningi cifukwa Gibeoni inali muzinda ukulu, monga umozi wamuzinda wa mfumu. Vnali ukulu kucila Ai, nabamvna bonse banali bankhondo bamphamvu. ³ Cifukwa cake Adoni - Zedeki, mfumu yaku Yelusalemu, anatuma wamtenga ku Honami, mfumu yaku Hebroni, ku Piram, mfumu yako Jaruta, ku Jaaphia, mfumu yako Lachish, na ku Debir, mfumu yaku Egloni: ⁴ "Bwela kulibe nakunithandiza ine. Tiyeni timenye Gibeoni cifukwa bapanga mtendele na Yoswa na bana ba Israyeli. ⁵ Mafumu yali (5) faivi ya Amoni, mfumu yaku Yelusalemu, mfumu yaku Hebroni, mfumu yaku Jarmuth, mfumu yaku Lachish, na mfumu yaku Egloni banabwela, beve nabonse bankhondo bao. Banakhala malo yao kunyamukila Gibeon, na kumumenya. ⁶ Bantu baku Gibeoni banatuma uthhenga ku Yoswa naba nkondo baku Giligala, Banakamba kuti, "yendesani! Osacosako manje yanu kuli mtumiki wanu bweleni ku ife mwamsanga na kuti pulumusa. Tithandizeni ise, popeza mamfumu yonse ya Amori bamene bakhala ma piri ya muziko bakumana pamozi kuti menya." ⁷ Yoswa anayenda ku giligala, iye nabonse bamuna ba nkondo na bonse bomenya nkondo. ⁸ Yehova anakamba kuli Yoswa, "osabayopa. Nabapasa mumanja yanu kulibe umozi pali beve azakulesa kumenya kwanu." ⁹ Yoswa anabwela pali beve mwazizizi, batayenda usiku bonse kucoka ku Giligala. ¹⁰ Yehova anasokonoza mudani pamenso ya Israyeli, Israyeli anabapaya na kukanthidwa kokulu pa Gibeoni na ku bapepeka panjila yoyenda ku Beth Horon, na kubapaya panjila yaku Azekah naku Makkedah. ¹¹ Pamene banali kuthaba Israyeli, pansi pa phili kucoka ku Beth Horon, Yehova anaponya miyala yakulu pansi kucoka kumwamba pali beve njira yonse paku ku Azekah, nipo anamwalila. Banali bambili banafa namatalala kucila banafa namapanga ya bamuna ba Israyeli. ¹² Pamenepo Yoswa anakamba na Yehova pasiku yamene Yehova anapasa bamuna ba Israyeli kupambana pali ba Amoni. Izi ndiye zamene Yoswa anakamba, "Zuba, imilila, pa Gibeoni, na mwezi, mu cigwa ca Aijalon." ¹³ Zuba ina imilila, na mwezi unaleka kuyenda paka ziko inabwezela cilango pali badani bao. Kodi izi sizinalembewe mu buku ya Jashar? Zuba inakhala mukati mwa mitambo; sinangena siku yonse. ¹⁴ Sukunankhalepe siku yatele kudala kapene kusogolo, pamene Yehova anamvelela mav ya banthu. Popeza Yehova anali kumenyelaka Israyeli nkondo. ¹⁵ Yoswa na Israyeli pamozi banabwelela kucigono ku Giligala. ¹⁶ Manje mafumu yali faivi yanathaba na kuzibisa mumakavu pa makkedah. ¹⁷ Zinabuziwa kuli Yoswa, "bapezeka! - mafumu yali faivi (5) yobisamu muma kavu ya makkedah!" ¹⁸ Yoswa anakamba kuti, kukhvnizilani miyala ikulu pakamba ka kavu nakvikapo basilikali kuti basungepo. ¹⁹ Osankhala imwe, pepekani badani banu na kubamenya ba mumbuyo. Osabavomekeza kungena mu mizinda yao, cifukwa Yehova mulungu wanu abapasa mu manja mwanu." ²⁰ Yoswa na bana ba Israyeli banasiliza kuba kantha nakukantha kukulu, paka banali pafupi kusililatu; Bang'ono cabe opulumuka banafika mizinda ya malinga. ²¹ Pamene gulu yonse yankhondo inabwelela mwamtendele kuli Yoswa ku cigono pa makkedah, kulibe wamene anayesa kukamba mav yamozi pali bana ba Israyeli. ²² Pamene Yoswa anakamba kuti, "segulani pakamwe ka kavu nakucosela mukavu mfumu zili faivi (5)." ²³ Banacita mwamene anakambila. Banamuletela mafumu yali faivi (5) kucoka mu kavu - mfumu ya Yelusalemu, mfumu yaku Hebron, na mfumu yaku Jarmuth, na mfumu yaku Lachish, na mfumu yaku Egloni. ²⁴ Ataleta mfumu kuli Yoswa, anaitana munthu alibonse wanu Israyeli. Anakamba kuli bakulu ba asilikali bamene banayenda kunkhondo nayeve, "fakani mapazi yanu pamikosi yabo." Pamene banabwela na kufaka mapazi yabo pamikosi yabo. ²⁵ Banakamba kuli beve, "osayopa na kuda nkhwana. Khalani okosa na mphamvu. Izi ndiye zamene Yehova azacita kuli badani bonse bamene muzamenyana nabo." ²⁶ Pamene Yoswa anamenya na kupaya mafumu. Anabapacika pamitengo zili faivi (5) anapacikiwa pamitengo paka mazulo. ²⁷ Pamene zuba inangena, Yoswa anapasa malamulo, nakubaselusa mumitengo naku bataila mu kavu kwamene benze banabisama. Banaika miyala yakulu pakamwaka kavu, miyala yaja yakalipo pakana lelo. ²⁸ Munjila iyi, Yoswa anatenga makkedah pasiku ija nakupaya alibonse muja napanga, kufakilako namafumu yabo. Anabonongelatu alibonse bokhalamo. sanasiyeko apulumuka alibonse. Acita kuli mfumu yaku makkedah mwamene anacitila kuli yaku Yeliko. ²⁹ Yoshuwa na yonse Israyeli inapita kuchoka ku Makedaya kuyenda ku Libina. Anayamba nkondo na Libina. ³⁰ Yehova anaipasa mumanja ya Israyeli-pamozi na mfumu yao. Yoshuwa anaononga na mupeni nakupaya muntu ali onse anali mo. Sanasiyemo muntu ali onse wamoyo. Anachita kuli mfumu yabo monga mwamene anachitila kuli mfumu ya Yeliko. ³¹ Ndipo Yoswa na Israyeli bonse anapitilila kucoka ku Libnah kuyenda ku Lachish. Anamanga misasa naku menya nkondo pamenepo. ³² Yehova anapasa Lachishi mu manja ya Israyeli, Yoswa anaitenga pasiku yacibili na kuikantha napanga ya kutwa na munthu alibonse okhalamo, mwamene anacitila ku Libnah. ³³ Pamenepo Horam, Mfumu yaku Gezer, anabwela kuthandiza Lachish. Yoswa anamenya iye paka kunalibe loko umozi opulumuka anasalako. ³⁴ Ndipo Yoswa na

Israyeli bonse bana pitila kucoka ku Lachish kuyenda ku Egloni. Banamanga misakasa nakumenya ziko ija,³⁵ nakuitenga siku yamene ija. Banaikantha na panga yakutwa na kubonongelatu alibonse okhala mo, mwamene Yoswa anacitila kuli Lachishi.³⁶ Ndipo Yoswa na Israyeli bonse banapitila kucoka ku Eglon kuyenda ku Hebroni. Banamenya nkhondo nayeve.³⁷ Banaitenga, nakvikantha napanga uakutwa, pamozi na mafumu yabo na mizi zao, nabanthu bonse bokhalamo. sibanasiyeko opulumuka, monga mwamene banacitila ku Egloni, banabonongelatu nabonse bokhalamo.³⁸ Pamenepo Yoswa anabwelela, naba nkhondo bonse ba Israyeli nayeve, nakupitila ku Debir na kumenya nkhondo nabeve.³⁹ Banaitenga, mfumu yabo na mizi yonse yapafupi. Banabakantha napanga yakutwa nakubonongelatu munthu alibonse bokhalamo. sibanasiyeko opulumuka. Banacita kuli Debir mwamene banacitila kuli Libnah na mfumu yabo na kuli Hebron.⁴⁰ Yoswa anakantha ziko yonse, ya kuma pili, ya kumwela, ya kumadimba na kuzigwa. pa mafumu yonse sanasiyeko alibonse opulumuka. Anabonongelatu ciliconse camoyo, monga mwamene Yehova, mulungu wa Israyeli, analamulila.⁴¹ Yoswa anabakantha kocokela ku kadesh Barnea mpaka ku Gaza, na maiko yonse ya ku Gosheni mpaka ku Gibeon.⁴² Yoswa anatenga mafumu yonse namalo yabo panthawi imozi cifukwa Yehova, mulungu wa Israyeli, anamenyela Israyeli.⁴³ Pamenepo Yoswa, na Israyeli bonse, banabwelela kucigono ku Giligala.

Chapter 11

¹ Pamene Jabini, mfumu yaku Hazor, anameela izi, anatuma uthenga kuli Jobab, mfumu yaku Madori, kuli mfumu yaku Shimron, nakuli Mfumu yaku Akshaph. ² Anatumansu uthenga kufuma yanali kumapili ya ku Mpoto kwaziko, mumana wa Yolodani kumwela kwa kinnereth, muzidikha, nakumitunda ya Dolo ku mazulo. ³ Anatumansu uthenga Akanani kumaa na ku ma zulo, ba Amoni, ba Hittites, ba Aperizi, ba Ayebusi mupili ya ziko, na ba Hivitesi pa phili ya Hermon mu ziko ya Mizpah. ⁴ Bonse bankhondo bao banacoka nabo, nambala ya ikulu yabasilikali, mu nambala monga dothi ya mumbali ya nyunja. Banali na nambala yaikulu ya akavalo na magaleta. ⁵ Yonse mafumu aya yanakumana panthawi yake, na kumanga pa manzi ya meloni kumenya nkhondo na Israyeli. ⁶ Yehova anakamba kuli Yoswa, "Osayopa pamenso yabo, cifukwa mailo panthawi iyi nibapasa bonse kuli Israyeli monga banthu bakufa. ⁷ Yoswa nabonse bamuna bankhondo banabwela. Banafika mwazizizi pamanzi ya meroni, nakumenya mudani. ⁸ Yehova anapasa mudani mumanja ya Israyeli, anabakantha nakuba pepekela kusidoni, misrephoth maim, na ku cigwa ca mizpah ku mawa. banabakantha pakana kulibe apulumuka vmozi anasala. ⁹ Yoswa anacita kuli beve monga Yehova anabavzila. Anadula akavalo na kushoka magaleta. ¹⁰ Yoswa anabwelela panthawi ija nakutenga Hazor. Anakantha mfumu yabo napanga. (Hazor ndiye anali mkulu wa mizi izi). ¹¹ Banakantha napanga ciliconse camoyo cinali muja, nakuvipatula kuti bavi bononge, ndipo kulibe ciliconse camoyo cinasiyiwa camoyo. Pamenepo anashoka Hazor. ¹² Yoswa anatenga mizinda yonse ya mafumu aya anatenganso mafumu yabo nakuya kanth napanga ya kutwa. Anaba bonogelatu napanga yakutwa, monga mwamene Mose mtumiki wa Yehova analamulila. ¹³ Israyeli sanashoke mizinda ili yonse yomangiwa pa zitunda, kucosaka Hazor. Yekha cabe anashoka. ¹⁴ Bankhondo ba Israyeli banatenga vonse votenga mizi pamozi na vobeta. Banapaya munthu alibonse napanga yakutwa pakana onse banafa sibansiye nyama yamoyo yopema. ¹⁵ Monga mwamene Yehova analamulila mutumiki wake Mose, munjila imozi, Mose analamulila Yoswa, na Yoswa anacita, sanasiyeko kalikonse kosacita ka mene Yehova analamulila Mose kucita. ¹⁶ Yoswa anatenga malo yonse: mapili yaziko, kumwela, malo yonse yau Gosheni, na ku madimba, mucigwa ca Yolodani, mapili ya ku Israyeli na ku madimba. ¹⁷ Kocokela kupili ya Halak pafupi na Edom, kupita ku mpoto kutali ku Gad mucigwa pafupi na Lebanoni pansi papili ya Hermoni, anatenga mafumu yonse na kubapaya. ¹⁸ Yoswa anamenya nkhondo kwanthawi itali na mafumu yonse. ¹⁹ Palibe muzinda umuzi unapanga mtendele na ba nkhondo ba Israyeli kucoselako ba Hivitesi banakhala mu Gibeori. Israyeli anatenga mizinda yonse munkhondo. ²⁰ Popeza ni Yehova anakosesa mitima yabo kuti bamenya nkhondo na Israyeli, kuti aba bonongeletu popanda cifundo, monga mwamene anapasila malamulo Mose. ²¹ Ndipo Yoswa anabwela panthawi ija nakubononga ba Anakimu. Anacita izi mupili yaziko pa Hebroni, Debir, Anab, na mupili ya Yuda, na mapi yaziko ya Israyeli. Yoswa anababonogelatu pamozi namizinda yabo. ²² Kulibe waba Anakimu anasiwa mumalo ya ya Israyeli kucosako pa Gaza, Gath na Ashdod. ²³ Pamene Yoswa anatenga malo, monga mwamene Yehova anakambila kuli Mose. Yoswa anapasa Israyeli monga cabo, Kupasiwa kumutundu vlibonse wao. Ndipo ziko inapumula kunkhondo.

Chapter 12

¹ Manje aya ndiye mafumu yamuziko, bamene bamuna bamu Israyeli banagonjesa. Ba Israyeli banatenga malo kumbali yakumawa kwa Yolodani kwamene zuba icokela, kucoka kucigwa ca mumana wa Aroni kufka ku phiri ya Hermoni, na konse ku Arabah kumawa. ² Sihon, mfumu ya Amoni, inankhala mu Heshbon. Anasogolela kucokela ku Aroer, yamene ili mumbali ya Arnon Gorge kucokela pakati ka cigwa, na pakati ya Gileadi kupita ku mumana wa Jabbok pamalile ya Amoni. ³ Sihon anajamulila pali Araban kufika kunyanja ya kinnereth, kumawa, kunyanja ya Arabah (nyanja ya mucele) kumawa! kuyenda ku Beth Jeshimoth na ku mwela, pansi poselukila phiri ya Pisgah. ⁴ Og, mfumu ya Bashani, mozi mwa opulumuka waba Rphaim, anakhala mu Ashtaroth na Edrei. ⁵ Analamulila pali phiri ya Hermoni, selekah, na konse ku Bashan, kumalile yabanthu ba ku Geshor na maacathites, na pakati ya Gilead, kumalile ya sihon, mfumu ya Heshbon. ⁶ Mose mutumiki wa Yehova, nabanthu ba Israyeli anabagonjesa, na Mose mtumiki wa Yehova, anapasa malo monga yabo kuli ba Alubeni, baGadites na pakati kamtundu wa manase. ⁷ Aya ndiye mafumu bamene Yoswa na banthu Israyeli banagonjesa kumbali yakumazulo kwa Yolodani, Kucokela ku Bar Gadi mucigwa pafupi na Lebanoni ku Phiri ya Halak pafupi na Edom. Yoswa anapasa malo kumitunda ya Israyeli kuti yakhale yabo beve. ⁸ Anabapasa mapili yaziko, ku cigwa, kumadimba, mbali yamapili, cipulu, na kumwela - malo ya ba Hittites, Amoni, Akanani, Apelezi, Ahivi, na Ayebusi. ⁹ Mafumu kufikilapo mfumu yaku Yeliko mfumu yaku Ai yamene ili pambali ya Beteli, ¹⁰ Mfumu ya Yelusalemu, mfumu ya Enaim, ¹¹ Mfumu yaku Jarmuth, mfumu yaku Lachish, ¹² Mfumu yaku Elgoni, mfumu ya ku Gezer, ¹³ Mfumu yaku Debir, mfumu yaku Gezer, ¹⁴ Mfumu yaku Hormah, mfumu yaku Aradi, ¹⁵ Mfumu yaku Libnah mfumu yaku Adullan, ¹⁶ Mfumu yaku Makkedah, mfumu yaku Beteli, ¹⁷ Mfumu yaku Tappuah, mfumu yaku Hepher, ¹⁸ Mfumu yaku Aphek, mfumu yaku Lasharoni, ¹⁹ Mfumu yaku Madon, mfumu yaku Hazor, ²⁰ Mfumu yaku Shimron, mfumu yaku Akshaph, ²¹ Mfumu yaku Taanach, mfumu yaku Megiddo, ²² Mfumu yaku Kedesh, mfumu yaku Jokneam Carmei, ²³ Mfumu yaku Dor mu Naphoth Dor, mfumu yaku Goyim mu Giligala, ²⁴ Mfumu yaku Tirzah, Nambala yamafumu inafeti wai (13) pamozi.

Chapter 13

¹ Manje Yoswa anakalamba pamene Yehova anakamba kuli yeve," wakalamba, koma kukali malo yambili yafunika kutenga. ² Aya ndiye malo yamene yakaliko: malile yonse ya Afilisti, nabonse ba Geshurites, ³ Kucoka ku shihor, kumawa kwa Eigipito, na kumpoto kwamalile ya Ekroni, ywmene itengewa monga katunda wa Akanani; Basogoleli bali faivi (5) ba Afilisti, baja baku Gaza, Ashdod, Ashkelo ni, Gath, na Ekroni - malo yaba Avvites. ⁴ Kuwela (malo ya Avvites); malo yonse ya Akanani, kucokela ku Arah yamene ipezeka ku sidonians, kutali kufika ku aphek yamene ili pamalile ya Amoni; ⁵ Malo ya ba Gebalites, Kulebanone konse kuyenda kumawa, kucoka ku Baal Gad pansi pa phili ya Hermon ko Lebo Hamath. ⁶ nakvikapo bonse bonkhala muphili yaziko kucoka ku Lebanoni kufika ku misrephoth maim, kuikako nabanthu bonse baku sidon. Nizacosa pamenso ya bankhaondo ba Israyeli. Onani kuti mupase malo kuli Israyeli monga yabo, mwamene ni nalamulila. ⁷ Gabani aya malo monga yanu yanu kumitundu yali naini (9) na mtundu bogabika wamanase." ⁸ Namutundu bogabika wina wamanase, A Rubeni, na ba Gadites banalandila malo yabo yamene Mose anabapasa kumbali yakumawa kwa Jolodani, ⁹ Kucokela Aroer, yamene ili mumbali mwa mumana wa Aroni (kuikako na muzinda uli pakati pa cigwa), naku cidikha conse ca medeba kufika ku Dibon; ¹⁰ Mizinda yonse yaku sihon, mfumu ya ba Amoni, analamulila mu Heshboni, kumalile ya Amoni, ¹¹ Gileadi, na malile ya Geshurites na malile ya Geshurites na maacathites, na phili yonse ya Hermoni, na Bashan yonse ku salekah; ¹² Naufumu bonse wa Og mu Bashani, amene analamulila mu Ashtaroth na Edrei - izi ndiye zina sula pali osala ba Rephaim - Mose anabakantha na kubacosa panja. ¹³ Koma banthu ba Israyeli sibanacose ba Geshurites kapena ba Maacathites. malo mwake, Geshur na maacath akhala pakati ka Israyeli lelo. ¹⁴ Kumutundu wa A Levi weka Mose sanapase coloba cao. zopeleka za Yehova, mulungu wa Israyeli, zopangiwa na muto, ndi coloba cabo, mwamene mulungu anakambila kuli Mose. ¹⁵ Mose anapasa coloba kumutundu wa A Rubeni, banja na banja. ¹⁶ Malo yabo yanali kuyambila ku Aroer, mumbali mwa mumana wa Aroni, na muzinda uli pakati pacigwa, na cidikha conse ca medeba. ¹⁷ Rubeni naye analandila Heshbon na mizinda yonse yali mu cidika, Dibon, na Bamoth Baal, na Beth Baal meon, ¹⁸ na Jahaz, na kedemoth, na mephaath, ¹⁹ na kiriathaim, na sibmah, na zereth shahar pa phili ya cigwa. ²⁰ Rubeni analandilanso beth peor, koselukila kwa pisgah Beth Jeshimoth, ²¹ Mizinda yonse ya ku cidikha, na ma ufumu yonse yaku sihon mfumu yaba Amoni, amene analamulila mu Heshboni, wamene Mose anagonjesa pamozi nabasogoleli ba midian, Evi Rekem, Zur, na Reba, kalonga wa sihon, amene anakhala mu ziko. ²² Bana ba Israyeli anapayafuti napanga Balaam mwana wa Beor, wamene anali kuombeza, pakati kabaja banapaya. ²³ Malile ya mutundu wa Rubeni ni mumana wa Yolodani; ndiye malekezero yabo. Ndiye cinali coloba ca Rubeni, kupasiwa kubanja iliyonse, namizinda zao na mizi zabo. ²⁴ Ndiye vamene Mose anapasa kumutundu wa Gadi, banja na banja; ²⁵ Malo yao yanali Hazer, mizinda yonse ya Gileadi na malo yoyabika ya Amoni, ku Aroer, yamene nikumawa kwa Rabbah, ²⁶ Kucokela ku Heshbon kufika ku Ramath mizpah na Betonim, kucoka ku mahanaim kufika ku malile ya Debir. ²⁷ Mucigwa, Mose anapasa Beth Haram, Beth Nimrah, succoth, na Zaphoni, na konse kwa ufumu wa sihon mfumu ya Heshboni, na Yolodani monga malile, kufika kosilizila kwa nyanja yaku kinnereth, kumawa kusogolo kwa Yolodani. ²⁸ Ndiye coloba ca mtundu wa Gadi, banja na banja, namizinda yabo na mizi yabo. ²⁹ Mose anapasa coloba ku mutundu bogabika wa manase. Inapasiwa kumutundu bogabika wa bana ba manase, banja na banja. ³⁰ Malile yabo yanayambila ku mahanaim, na Bashani yonse, na ufumu bonse wa Og wa Bashani na mizinda yaku jair, yamene yali mu Bashani, mizinda sikisite; ³¹ Gileadi bogabika, na Ashtaroth na Edrei (mitundu ya ufumu yaku Og mu Bashani). Aya yanapasiwa kubana ba makir mwana wa manase - banthu bogabika pakati ba makir, banja na banja. ³² Ndiye colowa camene Mose anapasa kuli beve kumadimba ya moabu, kupitilila Yolodani kumawa kwa Yeliko. ³³ Mose sanapase coloba kumutundu wa a Levi, Yehova, Mulungu wa Israyeli, ndiye coloba cabo, monga anakambila nabo.

Chapter 14

¹ Aya ndiye mbali ya malo yamene bana Israyeli banalandila monga coloba cabo muziko ya kanani, yamene Eleaza wa nsembe, Yoswa mwana wa Nuni, na basogoleli ba mitundu yamabanja ya Israyeli anabagambila. ² Coloba cabo cinasankhiwa na maele ku mitundu ili naini (9) na mutundu bogabika pakati, monga mwamene Yehova analamulila na zanja ya Mose. ³ Popeza Mose anapasa coloba ca mitundu ibilina mutundu vmozi bogabika pakati kupitilila Yolodani, koma kwa A Levi sanapase coloba. ⁴ Mutundu wa Yosefe yanali mitundu yabili, manase na Eflemu. A Levi sanapasiweko gabo yacoloba muziko, koma cabe mizinda yena ku khalamo, namalo ya vokudya ya vobeta vao na cuma cabo. ⁵ Bana ba Israyeli banacita monga Yehova analamulila Mose, ndipo banagawana malo. ⁶ Pamenepo mutundu wa Ayuda vnabwela kuli Yoswa pa Giligala. Calebu mwana Jephunneh mu kenizzite, anakamba kuli yeve, "uziba zamene Yehova anakamba kuli Mose munthu wa mulungu pali iwe na ine pa kadesh Barnea. ⁷ Ninali nazaka fote pamene Mose mtumiki wa Yehova ananituma kucoka ku kadesh Barnea ukabona malo. Ni Nbvesa mau kuli yeve monga cinali mumitima mwanga kupanga ⁸ Koma abale banga banayenda naine banalengesa mitima yabanthu kusungunuka na manthu. Koma ine ndina konka Yehova mulungu wanga na mtima wanga. ⁹ Mose analumbila siku ija, kukamba kuti, zoono malo yamene mapazi yayendamo yazakhala coloba cako na bana bako nthawi zonse, cifukwa wakonka Yehova mulungu wanga namtima wako bonse. ¹⁰ Manje ona! Yehova anasunga namoyo izi zako fote faivi (45), monga mwamene anakambila - kucukela nthawi yamene Yehova anakamba mau aya kwa Mose, pamene Israyeli anayenda mucipululu. manje, ona! siku yalelo nili nazaka eite faivi (85). ¹¹ Nikali na mphavu siku yalelo monga nenzeli musiku yamene Mose ananituma. mphavu zanga zili manje monga mwamene zinalilikale, za nkondo, za kuyenda na kubwela. ¹² Manje apa nipaseni iyi phili yaziko, yamene Yehova ananilonjeza pasiku ija. Popeza munamvela siku ija kuti ba Anakim banali kuja namizinda zikulu za malinga. cingakhale kuti Yehova azakhala naine nakuti nizaba cosamo, monga Yehova anakambila." ¹³ Oamene Yoswa anamudalisa na kumupasa Hebroni monga coloba kuli kalebu mwana wa Jephunneh. ¹⁴ Cifukwa cake Hebroni anakhala coloba cakalebu mwana wa Jephunneh mu kenizzite kufika siku yalelo, cifukwa anakonka Yehova, mulungu wa Israyeli na mtima wake bonse. ¹⁵ Manje zina ya Hebroni kali inali kiriath Arba. (Arba anali munthu mukulu pakati kaba Anakim) pamenepo malo yanapumula ku khondo.

Chapter 15

¹ Gabo yamalo yabanthu ba mtundu wa A Yuda, banja na banja, vkulila kumwela kumalile ya Edom, na cipulu ca zini kukhala kosilizila kumwela. ² Malile yabo kumwela yambila kumapeto ya nyanja ya mucele, kucoka ku bay (nyondo) yoyang'ana ku mwela. ³ Malile yabo yotulikila kumwela wacikweza ca Akraboim nakupitila ku zin, na kuyenda ku mwela wa kadesh Barnea, munjila pa Hezroni, na pamwamba ku Addar, kwamene upindamukila ku karka. ⁴ Vnayendela ku Azmon, nakucokela pa musinje wa Eigipito, nakubwela kosilizila pa nyanja. Ndiye yanali malile yabo yaku mwela. ⁵ Malile yakumawa yanali nyanja ya mucele, pakamwa pa Yolodani. Malile ku mpoto yayambila pa bay (nyondo) ya nyanja pakamwa pa Yolodani. ⁶ Inakwela ku Beth Hoglah na kupitila munjila kumpoto wa Beth Arabah. pamenepo inakwela kumwala wa Bohan mwana wa Rubeni. ⁷ Ndipo malile yanakwela ku Debir kucokela kucigwa ca Achor, na ku mbali ya ku mpoto kupindamukila ku Giligala, yamene ili pafupi na phili ya Adummim, yamene ili kumwela kwa cigwa. Ndipo malile yanapitila ku mazi ya En shemesh na kuyenda ku En Rogel. ⁸ Pamenepo malile yanakwela pa cigwa ca Ben Hinnom ku mwela wa muzinda wa Ayebusi (yamene ni Yelusalemu). Ndipo pacigwa ca Hinnoni, ku mazulo, ya, ene ili posilizila kupoto ligwa ca Rephaim. ⁹ Pamenepo malile yanakulila kuyambila pamwamba pa phili kufika kumazi ya Nephtoah, nakucoka kuja kuyenda kumizinda ya phili ya Ephron. Ndipo Malile yakoneka mozungulukaku Baalah (cimo zi mozi monga Kiriath Jearim). ¹⁰ Pamenepo malile yazungulila kumazulo ya Baalah kuphili ya Seir, na kupitila munjila kumbali ya phili Jearim ku mpoto (cimozi mozi monga kesalon) inayendela pansi ku cetu shemeth, na kupitila ku Timmah. ¹¹ Malile yanatulukila kumbali ya kumpoto ya phili ya Ekloni, na pamene munjila ya ku phili ya Baalah, kucoka paja inayenda ku Jabneel. malile ya nasilila panyanja. ¹² Malile yakumazulo yanali nyanja yaikulu na malile yake ndiye malile yozungulila mtundu wa Ayuda, banja pa banja. ¹³ Mukusunga lamulo ya Yehova kuli Yoswa, Yoswa anapasa kalebu mwana wa Jephunneh malo pakati pa mtundu wa A Yuda, kiriath Arba, yamene, Hebloni (Arba anali tate ba Anak). ¹⁴ Kalebu anatuluka kucoka naba batatu ba Anak: sheshai, Ahiman na Yalmali; bana ba Anaki. ¹⁵ Anayenda kucoka kuja kukonka bokhala baku Debir (Debir inali kuitaniwa kiriath sepher). ¹⁶ Kalebu anakamba kuti, munthu wamene amenya kiriath sepher na kuitenga, kuli yeve nizapasa Aksah mwana wanga mukuzi monga mkazi wake." ¹⁷ Pamene Othniel mwana wa kenaz, mubale wa kalebu, anaitenga, kalebu anapasa iye Aksah mwana wake monga mkazi wake. ¹⁸ Mwamusanga Zitapita izo, Aksah anabwela kuli Othniel na kumuza kuti apemphe munda kuli batate ake. pamene anaseluka pabulu wake, kalebu anakamba kuli yeve, "ufumu cani?" ¹⁹ Aksah anayankha, "nipaseni daliso, popesa mwanipasa malo yakumwela: nipasesoni visime vamazi." pamene kalebu anampasa visime vapamwamba na pansi. ²⁰ Ndiye cinali coloba ca mtundu wa Ayuda, banja pa banja. ²¹ Mizinda yakumutundu wa Ayuda kumaleke 10 ya kumwela, kufupi na malile ya Edom, yanali kabzer, Eder, Jagur, ²² Kinah, Dimonah, Adadah, Za ²³ Kadesh, Hazor, Ithman, ²⁴ Ziph, Telem, Bealoth, ²⁵ Hazoh Hadattah, Kerioth Hezroni (iyi inali kuitawanso kuti Hazoh), ²⁶ Amam, shem, moladah, ²⁷ Hazar Gaddah, Heshmon, Beth pelet, ²⁸ Hazar shual, Beersheba, Biziothiah. ²⁹ Baalah, Iyim, Ezem, ³⁰ Eltolad, Kesil, Hormah, ³¹ Ziklag, Madmannah, sansannah, ³² Lebaath, shilhim, Aim na Rimmon, Aya Yanali mizinda twenti naini pamozi, kufakilako mizi yabo. ³³ Mucigwa munali Ethtaol, Zorah, ³⁴ Zanaoh, En Gannim, Tappuah, Enam, ³⁵ Jarmuth, Adullan, Sokoh, Azekah, ³⁶ Shaaraimu, Adithaim na Gederah. (yamene ni Gederothaim) Aya yanali mizinda fotini (14) pamozi, kufakilako na mizi yabo. ³⁷ Zenah, Hadashah, Migdalgalad, ³⁸ Dilean, Mizpah, Joktheel, ³⁹ Lachish, Bozkath, Egloni, ⁴⁰ Kabbon, Lahmas, Kitlish, ⁴¹ Gederoth, Beth Dagon, Naamah, Makkedah. Aya yanali mizinda sikisitini (16) pamozi, kufakilako na mizi yabo. ⁴² Libnah, Ether, Asha, ⁴³ Iphtah, Ashnah, Nezib, ⁴⁴ Keilah, Akzib, Mareshah. Aya yanali mizinda yalli naini (9) pamozi, kufakilako mizi yabo. ⁴⁵ Ekloni, namizinda na mizi zozungulila; ⁴⁶ Kuyambila ku Ekloni kufika ku nyanja ikulu, na bonse benze kunkhala pafupi na Ashdod, kufakilako mizi yabo. ⁴⁷ Ashdod, mizinda yozungulila, kufakilako mizi yabo; Gaza, mizinda yazungulila kufakilako mizi yabo; paka ku musinje wa Eigipito, na ku nyanja ikulu namalile yake. ⁴⁸ Mu phili yaziko, shamir, Jattir, sokoh, ⁴⁹ Dannah, Kiriath sannah (yamene ni, Debir), ⁵⁰ Anab, Eshtemoh, Anim, ⁵¹ Goshen, Holon, na Giloh, Aya yana mizinda yali leveni (11) kufakilako mizi yabo. ⁵² Arab, Dumah, Eshani, ⁵³ Janim, Beth Tappuah, Aphekah ⁵⁴ Hvmtah, Kiriath Arah (yamene ni Hebloni), na Zior. Aya yanali mizinda yali naini (9) kufakilako mizi yabo. ⁵⁵ Maon, Carmel, Ziph, Tuttah, ⁵⁶ Jazreel, Jokdeam, Zanoah, ⁵⁷ Kain, Gibeah, na Timnah, Aya yanali mizinda yali teni (10) kufakiko mizi yabo. ⁵⁸ Halhul, Beth Zur, Gedor, ⁵⁹ Manrath, Anoth, na Eitekon. Aya yanali mizinda yali sikis (6), kufakilako mizi yabo ⁶⁰ Kiriath Baal (yamene ni, Kiriath Jearim), na Rabbah. Aya yanali mizinda yabili, kufakilako mizi yabo. ⁶¹ Mucipululu, munali Beth Arabah, Middin, Scacah, ⁶² Nibshana, muzinda wa mucele na E Gedi. Aya yanali mizinda sikisi (6) kufakilako mizi yabo. ⁶³ Koma kuli Ayebusi, bokhala mu Yelusalemu, mutindu wa A Yuda sanabacosemo, cifukwa cake Ayebusi akhala muja na mutundu wa Ayuda paka lelo.

Chapter 16

¹ Gabo ya malo ya mtundu wa Yosefe yanakulila kucoka ku Yolodani pa Yeliko, kumawa kwa cisime ca Yeliko, mucipululu, kuyenda kumwamba kucoka ku Yeliko kupitila muphili yaziko ya ku Beteli. ² Pamenepo inacoka ku Beteli kuyenda ku tuzi na kupitila njila yaku Adaroth, malo ya Arkites. ³ Ndipo inaselikila kumazulo kwa malo yaba Japhletites, kutali monga manga malo ya pansi Beth Horoni, na ku Gezer; inasilila pa nyanja. ⁴ Inali munjila kyi kuti mitundu ya Yosefe, manase na Eflemu yanalandila coloba cabo. ⁵ Malo ya mutundu wa Eflemu, banja pabanja; malila yacoloba cabo kumawa yanacokela ku Ataroth Addar kufika kumwamba kwa Beth horon, ⁶ nakucoka kuja inapitiliza kuyenda kunyanja. Kucoka ku mikmethath ku mpoto inakonekela kumawa kufupi na Taanath shiloh nakuipitilila kumawa kwa Janoah. ⁷ Pamenepo inayenda pansi kucoka ku Janoah kuyenda ku Ataroth na ku Naarah, na kufika pa Yeliko, kusilizila pa Yolodani. ⁸ Kuyambila ku Tappuah malile yana yenda kumazulo kwa musinje wa kanah naku silizila pa nyanja. Ndiye cinali coloba ca Eflemu, banja pa banja, ⁹ Pamozi namizinda yamene yanasankhiwa yamitundu ya Eflamu pamozi na coloba ca mutundu wa manase mizinda yonse kufukilako mizi zao. ¹⁰ Sabanacose Akanani bamene banakhala mu Gezer kuti Akanani akhala pakati ka Eflamu kufika lelo, koma banthu bana pangiwa kupapa mokaka miziwa.

Chapter 17

¹ Iyi ndiye inali yabo ya malo ya mutundu wa manase (Amene anali mwana boyamba wa Yosefe) - yamene, niya makir, wamene anali mwana boyamba wa manase na wamene yeve anali tate wa Gileadi. Bana ba makir banapasiwa malo ya Gileadi na Bashani, cifukwa makir anli munthu wankhondo. ² Malo yanapasiwa kul munthu bosala wa manase, kupasiwa kuli mabanja yabo - Abiezer, Kerek, Asriel, shechem, Hepher, na shemida. Aba banali bana bamuna ba manase mwana wa Yosefe, monga mwabanja yabo. ³ Manje, zelophehad mwana wa Hepher mwana wa Gileadi mwana wa makir mwana manase analibe bana bamuna koma bakazi cabe. Mazina yabana bakazi yanali mahlah, Noah, Hoglah, Milkah, na Tirzah. ⁴ Anabwela kuli Eliyaza wansembe, Yoswa mwana wa Nuni, naba sogoleli, nakukamba kuti, "Yehova analamulila Mose kutipasa coloba pamozi na babale banthu." Ndipo, kukonka cilamulo ca Yehova, anapasa azimai baja coloba pakati ka bale batate bake. ⁵ Magabo yali teni (10) yamalo yanapasiwa kuli manase mu Gileadi na Bashani, yamene ili ku mbali ina ya Yolodani, ⁶ Cifukwa bana bakazi ba manase banalandila coloba pamozi nabana bamuna. malo ya Gileadi yanapasiwa kuli bana bosala ba manase. ⁷ Malo ya manase yanafika kucoka pali Asha kufika ku mikmethath, yamene ili kumawa kwa shachem. Pamenepo malile yanayenda kubwela kuli baja bokhala pafupi na cisime ca Tappuah. ⁸ (Malo ya Tappuah yanali ya manase, koma muzinda wa Tappuah pa malile ya manase yanali ya banthu ba Eflemu). ⁹ Malile yanapita pansi kumusinje wa kanah. Aya mizinda yamisinje pakati pa mizinda ya manase yanali ya Eflemu. Malile ya manse yanali ku mpoto ya ku musinje, ndipo inasilila panyanja. ¹⁰ Malo yako mwela yanali ya eflemu, na malo ya ku mpoto yanali ya manase; nyanja inali malile. Kumbali ya ku mpoto angakumane na Asha na kumawa, Issachar. ¹¹ Namuli Issacha na Asha, manase anatenga Beth shana mizi yabo, Ibleam na mizi yabo, bokhala mu Dor na mizi yake, bokhala bamu Fndor na mizi yabo, bokhala bamu Taanach na mizi yake, na bokhala baku megiddo namizi yabo (na muzinda wacitatu ni Napheth). ¹² Koma mutundu wa manase sunatengeko mizinda yaja, popeza Akanani anapitiliza kukhala malo. ¹³ Pamene bantu ba Israyeli banakula mphavu, banaika ba kanani kupapa kwacika kamizo, koma sanabaco selemotu. ¹⁴ Pamenepo bana ba Yosefe anakamba kuli Yoswa, kuti, "cifukwa cani watipa cabe yabo imozi ya malo na mbali imozi ya coloba, papeza ndife banthu bambili ngako, na kudala Yehova atidalisa?" ¹⁵ Yoswa anakamba kuli beve, "ngati ndimewe banthu bambili, yenda musanga nakukonza minda yanu mu malo ya Aperezi na ba Rephaim. Cipani ici popeza phili yaziko ya Eflemu niyai ng'ono kuli imwe. ¹⁶ Bana ba Ysefe banakamba kuti, "phili ya ziko siyingakwanile ise. koma ba kanani bonse bamene banakhala mucigwa ali namagaleta ya nsimbi, bonse bamene bali mu Beth shani na mizi yabo, na baja bali mucigwa ca Jezreal." ¹⁷ Pamenepo Yoswa anakamba kunyuma ya Yoswa - kuli Eflemu na manase, " ndimwe banthu bambili munambala, nakuti muli na mphavu zikulu. simufunika kukhala cabe na malo yamozi yokupasani. ¹⁸ Phili ya ziko izi khalanso yanu, nangu nisanga, muzalimapo nakutengo kufika kumalile yakutali. Muzacosamo Akanani ingakhale bali namagaleta ya nsimbi, nangu ni ba mphavu."

Chapter 18

¹ Ndipo musonkano bonse wa bana ba Israyeli banakumana pamozi pa shiloh. Banaika cihema cokumanilamo paja nakugonjesa malo pamenso pabo. ² Panali mitundu ili seveni pakati kabana ba Israyeli bamene coloba cabo sicina gabwe. ³ Yoswa anakamba ku bana ba Israyeli kuti, "mucebwa paka liti kungena mumalo yamene Yehova, mulungu wamakolo yanu, akupasani?" ⁴ Zisankhileni bamuna batatu kucoka kumutundu ulibonse, ndipo nizabatuma. Bazayenda nakubona malo pamwamba napansi. Bazalembe mwamene bayabo nela mwa coloba cabo, nakubwelelanso kuli ine. ⁵ Bazaigaba magabo yali seveni. Yuda azasala mu malo yabo ku mwela, na nyumba ya Yosefe iza pitiliza mumalo ya mpoto. ⁶ Uzalembe malo muzigabo zili seveni na kuleta zolembe kuli ine. Nizacita muele yanu pamanso ya Yehova mulungu wanu. ⁷ Alevi alibe gabo pakati panu, popeza unsembe wa Yehova ndiye coloba cabo. Gadi, Rubeni, na mutundu bgabika lva manase evalandila coloba cabo, kupitilila Yolodani. Ndiye coloba camene Mose mutumiki wa Yehova anabapasa." ⁸ Ndipo bamuna bananyamuka nakuyenda, Yoswa analamulila baja banayenda kulemba maonekedwe yamalo, kukamba kuti, "yendani kumwamba na pansu mu malo nakulemba mwamene yabonekela nakubwelela kuli ine. Nizacitila imwe maele pano pamene ya Yehova pa shiloh. ⁹ Bamuna banayenda nakuyenda - yenda pamwamba na Pansi mu malo na kulemba maonekedwe mubuku mwa mizinda yake muzigabo zili seveni, kulemba mizinda mucigabo ciliconse. pamenepo banabwelela kuli Yoswa mucigono ca shiloh. ¹⁰ Pamene Yoswa anabacitilako maele pashiloh pamenso ya Yehova. pansu paja kuti Yoswa anagabila malo bana ba Israyeli, kui alibonse anapasiwa gabo ya malo. ¹¹ Kugaba kwa malo ya mutundu wa Benjamini banja pa banja. malile yamalo yabo yogabiwa yanali pakati pa bana ba Yuda bana ba Yosefe. ¹² Kumbali yako mpoto, malile yabo yayambila pa Yolodani. malile yabo yanakwela kumumpoto kwa Yeliko, na kumwamba kupitilila muphili ya ziko kumazulo. kuja inafika mucipululu ca Beth Aven. ¹³ Kucokela kuja malile yanapitila ku mwela kunjila ya Lvz (malo yamozi monga Beteli) pamenepo malile ili kumwela kwa Beth Holoni. ¹⁴ Malile pamenepo yanayenda njila ina; kumbali ya kumazulo inakonekela ku mwela, kuyenda ku ma phili kusogolo kwa Beth Holoni. Aya malile yasilila pa kiriath baal (yamene, ni kiriath Jearim), muzinda unali wa mutundu wa Ayuda. Ici cinapanga malile ku mbali yaku mazulo. ¹⁵ Mbali ya ku mwela inayambila kunja kwa kiriath Jearim. Malile yanacokela kuja kuyenda ku Ephroni, ku cisime camanzi ya Nephtoah. ¹⁶ Malile pamenepo yanayenda pansu kumalile ya cigwa ca Rephaim. ndipo inayenda pansu ku cigwa ca Hinnom, kumwela koselukila kwa Ayebusi, na kupitilila pansu ku En Rogel. ¹⁷ Inakonekela kumpoto, kuyenda njira yaku En shemesh, nakucoka kuja inacoka kuyenda ku Geliloth, yamene inali pafupi na Adummim. pamenepo inayenda pansu ku mwala wa Bohan mwana wa Rubeni. ¹⁸ Inayendela kumu mpoto kwa Beth Araba na pansu ku Araba. ¹⁹ Malile yanayenda kumbali ya ku mpoto kwa Beth Hoglah. Malile yanasilila kumwela wa nyanja ya mucele, posilizila Yolodani kumwela. Aya ndiye yanali malile ku mwela. ²⁰ Yolodani inapanga malile yake kumbali yakumawa. Ndiye cinali coloba ca mtundu wa Benjamini, ndipo cinapasiwa ku banja na banja, malilena malile, mo zungulila. ²¹ Manje mizinda yamitundu ya Benjamini, banja na banja, yanali na mizinda aya: Yeliko, Beth Hoglah, Emek kaziz, ²² Beth Arabah, Zemaraim, Beteli, ²³ Avvim, Parah, Ophrah, ²⁴ Kephrah Ammoni, Ophni, na Geba, Tanali mizinda tyovv (12) kafakilako mizi yabo. ²⁵ Kunalinso mizinda ya Gibeon, Ramah, Beeroth, ²⁶ Mizpah, Kephrah, Mozah, ²⁷ Rekem, Irpeel, Taralah, ²⁸ Zelah, Haeleph, Jebus (cimozi mozi monga Yelusalemu), Gibeah, na Kiriath yanali mizinda fotini, kufakilako mizi yabo. Ndiye cinali coloba ca Benjamini ca mabanja yabo.

Chapter 19

¹ Kucita kwamaele kwacibili kunagwela pali simiyoni, banja pa banja. coloba cabo cinali pakati ka coloba ca Ayuda. ² Coloba cabo cina Beersheba, Sheba, Moladah, ³ Hazar Shual, Balah, Ezem, ⁴ Eltolad, Bethul, na Hormah, ⁵ Simiyoni analinso na Ziklag, Beth Markaboth, Hazar Susah, ⁶ Beth Lebaoth, na Shauhen, Aya yanali mizinda fetini (13), kafakilako na mizi yabo. ⁷ Simiyoni analinso na Ain, Rimmon, Ether, na Ashan. Aya yanali mizinda fo (4) kafakilako na mizi. ⁸ Aya yanali pamozi, kufakilako na mizi yabo yozungulila mizinda kufika ku Baalath Beer (cimozi mozi monga Ramah ku mwela). Ndiye cinali coloba ca simiyoni, banja na banja. ⁹ Coloba camutundu wa Simiyoni cinapanga mbali ya malo ya mutundu wa Yuda. Cifukwa gabo yamalo inapasa ku mtundu wa Yuda yanali yakulu kuli beve, mutundu wa Simiyoni unalandila coloba cabo kucoka pakati pa gabo yabo. ¹⁰ Maele yacitatu yanagwela pali Zebulun, banja na banja, malile ya coloba cabo yanayambila pa Sarid. ¹¹ Malile yanapita kuwamba kumazulo kwa Maralah na ku gusa Debesheth; pamenepo yanakulila ku musinje unali pafupi na Jokneam. ¹² Kucokela ku Sarid malile yanakoneka ku mawa ku yenda kumawa kumalile kisloth Tabor. Kucokela uko yanayenda ku Daberth nakuyenda ku Japhia. ¹³ Kucoka uko yanayendela kumawa kwa Gath Hepher, na kuyenda ku Eth kazin; cokokapo yanayenda ku Rimmon na kukonekela ku Neal. ¹⁴ Malile yanakonekela ku mpoto ku Hannathon na ku silila pa cigwa ca Iphtah Ei. ¹⁵ Ici cigabo kufakilako mizinda ya kattath, Nahalal, Shimron, Idalah, na Bethlechemo. Yanali mizinda tyovv(12) pamozi, kafakilako mizi yabo. ¹⁶ Ndiye cinali coloba camutundu wa zebulun, banja na banja, mizinda aya, kufakilako mizi yabo, ¹⁷ Maele ya namba fo (4) yanagwela pa Issacah, banja na banja. ¹⁸ Malo yabo kafakilako Jezreel, Chesulloth, Shunem, ¹⁹ Hapharaim, Shion na Anaharath. ²⁰ Inaikilako na Rabbith, Kishion, Ebez, ²¹ Remeth, En Gannim, En Haddah, na Beth pazez. ²² Malile yabo yana Tabor, Shahazumah, na Beth Shemesh, nakusilila pa Yolodani. Tanali mizinda sikisitini (16) kufakilako mizi yabo. ²³ Ndiye cinali coloba ca mutundu wa Issachah, kulingana na banja yabo - mizinda, kafakilako mizi yabo. ²⁴ Maele yanamba faivi (5) yanagwela pali mtundu wa Asha, banja na banja. ²⁵ Malo yabo kufakilako Helkath, Hali, Beten, Akshaph, ²⁶ Allammeleki, Amad, na mishall, ku mazulo malile yanakulila ku carmel naku shihor Libnath. ²⁷ Pamenepo yanakonekela kumawa ku Beth Dagon na kuyenda kutali monga ku Zebulun, na kuyenda ku cigwa ca Iphtah El, kumpoto ku Beth Emekina Neiel. ²⁸ pamenepo yanapitiliza ku kabul ku mpoto. Ndiye inapita ku Abadon, Rehob, Hammon, na Kanah, kufaka ku sidon yaikulu. ²⁹ Malile yanabwelela ku Ramah, nakuyenda kumizinda wa malinga wa Tyre. pamenepo malile yanakonekela ku Hosah nakusilila panyanja, mucigabo ca Akzib. ³⁰ Ummah, Apheki, na Rehob. Yanali mizinda yali twenti thu (22), kufakilako mizi yabo. ³¹ Ndiye cinali coloba ca Asha, banja na banja - mizinda, kafakilako mizi yabo. ³² Maele ya namba sikisi (6) yanagwela pali mutundu wa Naphtali banja na banja. ³³ Malile yabo yayambila ku Heleph, kucoka ko Oak pa Zaanannim, kufaka ku Adami Nekeb na Jabneel, kufika ku Lakkvm; inasilila pa Yolodani. ³⁴ Malile yanakonekela kumazulo kwa Aznoth Tabor na kuyenda ku Hukkok; inagusa Zebulun ku mwela, na kufika kuli Asha kumazulo na kuli Yuda kumawa kwa mumana wa Yolodani. ³⁵ Mizi yobisamamo yanali Ziddim, Zer, Hammath, Rakkath, Kinnereth, ³⁶ Adamah, Ramah, Hazor, ³⁷ Kadesh, Edrei, na En Hazor. ³⁸ Kunalinso Yironi, Migdal El, Horem, Beth Anath, na Beth shemesh. Yanali mizinda yali naintini (19) kafakilako na mizi yabo. ³⁹ Ndiye cinali coloba ca Naphtali, banja na banja mizinda, kufakilako na mizi yabo. ⁴⁰ Maele ya namba seveni yanagwela pa mtundu wa Dani, banja na banja. ⁴¹ Malo ya coloba cake kufakilako Zorah, Eshtaol, Ir shemesh, ⁴² Shaalabbin, Aijaloni, na Ithlah. ⁴³ Inakilako na Eloni, Timnah, Ekroni, ⁴⁴ Eitekeh, Gibbetho, baath, ⁴⁵ Jehud, Bene Berak, Gath Rimmon, ⁴⁶ Me Jarkon, na Rakkon pamozi namalo yakusogolo kucoka ku Joppa ⁴⁷ Pamene malo ya mutundu wa Dani yanasoba kuli beve, Dani anamenya Leshem, kumenyana nayo, kuitenga nakuilasa napanga; kuitenga naku khalamo. Banapasa futi Leshem zina, kuitana Dani pa zina ya makolo. ⁴⁸ Ndiye cinali coloba mutundu wa Dani, banja na banja, kufakilako mizi yabo. ⁴⁹ Pamene banasiliza kupasa kwa malo monga coloba bana ba Israyeli banapasa coloba pakati kabo kuli Yoswa mwana wa Nuni. ⁵⁰ Mwa cilamulo ca Yehova banamupasa muzinda wamene anapempha, Timnath Serah mu phili yaziko ya ku Eflamu. Anamanganso muzinda nakukhalamo. ⁵¹ Izi ndiye zoloba zamene Eliyaza wa nsembe, Yoswa mwana wa Nuni, naba sogoleli ba mitundu yabanja ya Israyeli yanapasiwa na maele pa shilo, pamenso ya Yehova, pakhomo ya cihema cokumanilamo. Ndipo anasiliza kupasa malo.

Chapter 20

¹ Pamene Yehova anakamba kuli Yoswa, ² "kamba ku bana ba Israyeli, kuti sanku mizinda yo pulumukilamo yamene ninakamba naiwe na kwanja kwa Mose. ³ Cita ici kuti wamene apaya munthu mosaziba anga yenda kuja. Aya mizinda yazakhala malo yopulumukilamo kuli alibonse amone afuna magari yamu nthu anapaiwa. ⁴ Azathabila kumuzinda vmozi nakuimilila pongenela khomo ya muzinda, nakukamba mulandu wake kulu bakulu ba muzinda. Pamenepo bazangenesa mu mzinda nakumuuoasa malo yake kukhala pakati kabo ⁵ Ngati vmozi pali beve afuna magari ya munthu anapaiwa, Ndipo banthu bamumzinda basapeleka uja anamupaya kuli olamulila. sibafunika kucita izi cifukwa anapaya muzake cosaziba, nakuti analiba cizondo kuli yeve kudala. ⁶ Afunika kunkhala mumzinda paka aimilile pasogolo paciwevzo, paka omfa yauja anali kutumikila monga wansembe mkulu masiku yaja. Pamenepo buja amene anapaya mwangozi munthu angabwelela ku mzinda wake na ku numba yake kwamene anathaba. ⁷ Bana ba Israyeli banasankha kadesh mu Galileya muphili yaziko yaku Naphtali, shechem muphili yaziko yaku Eflamo, na Kiriath Arba (cimozi mozi monga Hebroni) mu phili ya ziko ya Ayuda. ⁸ Kupitila Yolodani kumawa kwa Yeliko, banankha Bezer mu cipululu pa cidikha kucoka ku mutundu wa Rubeni, Ramoth Gileadi, kucoka kumutundu wa Gadi; na Golani mu Bashani, kucoka kumutundu wa manase. ⁹ Aya ndiye mizinda yanasankhiwa ya bana ba Israyeli na yabalendo bamene bakhala pakati pabo, kuti alibonsenanapaya munthu cosaziba angathabileko na kupulumukilako. Uyu munthu sazamalila na kwanja kwa munthu enze kufuna magari yamene yanacoka, paka uja munthu wamujandu coyamba aimilila pa msonkhano.

Chapter 21

¹ Pamenepo basogoleli ba mutundu wa Alevi bana bwela kuli Eliyaza wansembe, kuli Yoswa mwa wa Nuni, nakubasogoleli bamabanja yamakolo yabo pakati kabana ba Israyeli. ² Banakamba kuli beve pa shilo muziko yakenani, "Yehova analamulila iwe pa kwanja kwa Mose kupasa kuli ise mizinda yonkhalamo, ndi mabusa ya vobeta vathu." ³ Ndipo mwacilamulo ca Yehova, bana ba Israyeli banapasa coloba cabo kumizinda aya, kufakilako mabusa yabo, kuli ALevi. ⁴ Kucita kwa maele kwama banja ya kohathites yanapasa izi, Bansembe - bana ba Aaroni bamene bana coka kuli ALevi - banalandila mizinda fetini (13) kucoka kumutundu wa Ayuda, kucoka kumutundu wa simiyoni, kucoka kumutundu wa Benjamini. ⁵ Bana bosala ba kohath banapasiwa mizinda yali teni kucoka kumabanja yamutundu wa Eflemu, Dani, na kumutundu bogabika wamanase. ⁶ Pamenepo banthu bocokela mubanja ya Gershon banapasiwa, mwakucita maele, mizinda yali fetini (13) yocokela kumabanja ya mutundu wa Issachar, ASELI, Naphtali, na mutundu bogabika pakati wa manase mu Bashani. ⁷ Banthu banali bana ba Merari, banja pa banja, banalandila mizinda tyovu (12) kucokela kumutundu wa Rubeni, Gadi, na Zebuluni. ⁸ Motelo bana ba Israyeli banapasa, pakucta maele, mizinda aya (kufakilako mabusa yabo) kuli ALevi, monga mwamene Yehova analamulila mwa kwanja kwa Mose. ⁹ Kucokela kumutundu wa Yuda na simiyoni, banapasa malo kumizinda aya, aya yolembewa mwa mazina yabo. ¹⁰ Aya mizinda yanapasiwa kuli bana ba Anroni, yamene yanali pakati pa mabanja ya kohathitesa, yamene yanali kucoka kumutundu wa Levi. pakuti maele boyamba yanagwela pali beve. ¹¹ Bana ba Israyeli banabapasa kiriath Araba (Arba analitate wa Anak), malo yamozi - mozi monga Hebroni, mu phili ya ziko ya Yuda, na mabusa yozungulila. ¹² Koma minda yamumizinda, kafakilako mizi zayo, yanapasiwa kuli kalebu mwana wa ya Jephumehe, monga cuma cake. ¹³ Kubana ba Anroni wasembe banapasa Hebroni na mabusa - yamene unali muzinda bopulumukilamo ya alibonse anapaya wina cosaziwa - na Libnah na mabusa yabo, ¹⁴ Jattir na mabusa yake, na Eshtemoa na mabusa yake. ¹⁵ Banapanso Holoni na mabusa bake, Debir na mabusa ake, ¹⁶ Ain na mabusa yake, Juttah na mabusa, na Beth shemeth na mabusa yake. Panali mizinda yali naini (9) yamene yanapasiwa kucokela kumutundu yabili. ¹⁷ Kucokela kumutundu wa Benjamini banapasiwa Gibeoni na mabusa yake, Geba na mabusa yake, ¹⁸ Anathoth na mabusa yake, na Almoni na mabusa yake na mizinda inai. ¹⁹ Mizinda yopasiwa kuli bansembe, bana ba Aaroni, yana fetini pamozi, kufakilako mabusa yabo. ²⁰ Kuli osala ba kohathites bucokela ku kumabanja ya ALevi - banali na mizinda yanapasiwa kuli beve kucoka kumutundu wa Eflemu mwakucita mwaele. ²¹ Kuli beve kunapasiwa shecheme na mabusa yake muphili ya ziko ya Eflemu - muzinda wopulumukilamo ya alibonse anapaya cosaziba - Gezer na mabusa yake, ²² Kibzaim na mabusa yake, na Beth Horoni na mabusa yake - mizinda fo (4) pamozi. ²³ Kucoka kumutundu wa Dani, banja ya kohath ya napasiwa Eltekeh na mabusa yake, Giibbethon na mabusa bake, ²⁴ Aijaloni na mabusa yake, na Gath na mabusa yake - mizinda yanai (4) pamozi. ²⁵ Kucoka kumutundu bogabika wa manase, banja ya kohath, inapasiwa Taanach na mabusa yake na Gath kimmo na mabusa yake - mizinda ibili. ²⁶ Munali mizinda ili teni mumabanja yonse yasalaya kohathites, kufakilako mabusa yabo. ²⁷ Kucoka kumutundu bogabika pakati wa manase, ku mabanja ya Gershon, aya yanali mabanja yena ya Alevi, ndipo banapasa Gulani mu Bashani na mabusa yake - muzinda bopulumukilamo wa alibonse anapaya muzake cosaziba, pamozi na Be Eshterah na mabusa yake - mizinda ibili pamozi. ²⁸ Kumabanja ya Gershoni banapansanso kishion kucoka kumutundu wa Issachar, pamozi na mabusa yake, Deberath na mbausa yake, ²⁹ Jarmuth na mabusa yake, na En Gannim na mabusa yake - mizinda fo (4). ³⁰ Kucoka kumutundu wa Aseli, banapasa mishal namabusa yake, Abadoni na mabusa yake, ³¹ Helkath na mabusa yake, na Rehob na mabusa yake, mizinda ili fo (4) pamozi. ³² Kucoka kumutundu wa Naphtali, banapasa mabanja ya Gershoni kadesh mu Galiteya na mabusa yake, muzinda bopulumukilamo wa alibonse anapaya cosaziba; Hammoth por na mabusa yake, na Kartun na mabusa yake - mizinda itatu pamozi. ³³ Yanali mizinda fetini (13) pamozi, kucoka mumabanja ya Gershoni, kufakilako mabusa yabo. ³⁴ Kuli ALevi busala - mabanja ya merari - banapasiwa kucoka kumutundu wa zebuluni: Jokneam na mabusa yake, kartah namabusa yake, ³⁵ Dimnah na mabusa yake, na Nahalal na mabusa yake mizinda yali fo (4) pamozi. ³⁶ Kumabanja ya merari banapasiwa kucoka kumutundu wa Rubeni Bezer na mabusa yake, jahazi na mabusa yake. ³⁷ Kedemoth na mabusa yake, na mephaath na mabusa yake - mazinda ili fo (4). ³⁸ Kucoka kumutundu wa Gadi banapasiwa Ramoth mu Gileadi na mabusa yake - muzinda pulumukilamo wa alibonse anapaya wina cosaziba - na mahanaim na mabusa yake. ³⁹ Mabanja ya merari yanapaswanso Heshboni na mabusa yake, na jazer na mabusa yake, Aya yanali mizinda yali fo (4) pamozi. ⁴⁰ Yonse aya yanali mizinda yamabanja yosiyana - siyana ya merari, yanali kucokela kumutundu wa ALevi - mizinda zili tyow (12) pamozi zinapzsiwa kuli beve mwakucita maele. ⁴¹ Mizinda ya ALevi yotengewa pakati ka malo yatengewa na bana ba Israyeli yanali mizinda fote eiti (48), kufakilako na mabusa yabo. ⁴² Aya mizinda ili yonse yenze na mabusa yazungulila, zenze so chabe namizinda yonse. ⁴³ Pamenepo Yehova anapasa

Israyeli malo yonse yamene analumbilila kupasa kumakolo yabo, bana ba Israyeli banayatenga naku nkhalamo.

⁴⁴ Pamenepo Yehova anabapasa kupumula mbali zonse, monga mwamene analumbilila kumakolo yabo. Kulibe lukumudani umozi anabagunjesa. Yehova anapasa bonse badani bao mumanja yabo. ⁴⁵ Kunalibe cimuzi pali malonjezo yonse yamene Yehova anakamba kunyumba ya Israyeli yanakanga kucitika.

Chapter 22

¹ Panthawiinja, Yoswa anaitana Arubeni, A Gadites, na mutundu bogabika pakati wa manase. ² Ananakamaba kuli beve," mwacita vonse vamene Mose mutumiki wa Yehova anakulamulila iwe, wamvelela mau yanga mu vonse nina kulamulila. ³ Sunasiye abale ako masiku aya, paka kufika nalelo, na kukwanilisa nchito zofunika mwa malamulo ya Yehova mulungu wanu. ⁴ Manje Yehova mulungu wako apasa kupumula kuli abale bako, monga mwamene anabalonjezela. cifukwa chake bwelelani nakuyenda kumahema yanu mu malo yanu, yamene Mose mutumiki wa Yehova anakupasani kumbali ina ya Yolodani. ⁵ Khalani bo bonesesa kukonkha malangizo na namalamulo yamene Mose mutumiki wa Yehova anakulamulila iwe, kukonda Yehova mulungu wako, kuyenda munjila zake zonse, kusunga malamulo yake yake, nakulamulila kuli yeve na kumulambila namitima wako bonse na moyo wako bonse." ⁶ Pomwepo Yoswa anabadalisa na kubatuma, ndipo banabwelela ku mahema yabo. ⁷ Manje kuli imozi ya mutundu bogabika pakati wa manase Mose anapasa coloba mu Bashani, koma kumbali ina Yoswa anapasa coloba pambali namubale wabo mumalo yakumazulo kwa Yolodani. Yoswa anababuza kuti bayende kumahema yabo; anabadalisa ⁸ nakukamba nabeve," bwelelani kumahema yanu na ndala zambili, na vobeta vambili, na siliva na Golide, na Bronzi na nsimbi, na vovala vambili. Gabana votenga kuli badani banu na ba bale banu. ⁹ Ndipo bana ba Rubeni, bana ba Gadi, na mutundu bogabika pakati wa manase unabwelela kunyumba, kusiya banthu ba Israyeli pa shiloh, yamene ili muziko ya kanani. Banacoka kuyenda kucigabo ca Gileadi, kumalo yabo, yamene beve banatenga, mukumcelela kulamulo ya Yehova, mwa kwanja kwa Mose. ¹⁰ Pamene banabwela ku Yolodani yamene ili muziko ya kanani, A Rubeni na ba Gadites na mutundu bogabika pakati wa manase unamanga guwa pambali ya Yolodani, guwa yaikulu yamaonekedwe yabwino. ¹¹ Bana ba Israyeli banamvela pali ivi nakukamba kuti," ona! banthu ba Rubeni, Gadi, na mutundu bogabika pakati wamanase bamanga gua kusogolo kwaziko yakanani, pa Geliloth, mucigabo pafupi na Yolodani, kumbali ya bana ba Israyeli." ¹² Pamene bana ba Israyeli bana mvela pali ici, musonkhano bonse bwa banthu ba Israyeli unakumana pamozi pa shiloh kuyenda kuwamba kukamenya nkondo nabeve. ¹³ Ndipo bana ba Israyeli banatuma amithenga kuli A Rubeni, A Gadites, na mutundu bogabika pakati wa Manase, mumalo ya Gileadi. Banatumanso phlnehasi mwana wa Eliyaza, wa nsembe, ¹⁴ Pamozi nabosogoleli bali teni (10) umozi kucokela kumutundu wa mabanja ya Israyeli, na alibonse wa beve anali musogoleli wabanja pakati ka mabanja ya Israyeli. ¹⁵ Banabwela kuli bana ba Rubeni, Gadi, na mutundu bogabika pakati wa manase, muziko ya Gileadi, ndipo anakamba nabeve: ¹⁶ Musonkhano bonse wa Yehova ukamba izi, 'nicani ici cosa khulupililika camene wacitila mulungu wa Israyeli, pakucinja munjila iyi siku yalelo kuleka kukonka Yehova na kuzimangila imwe mweka guwa lelo yo bukila mulungu? ¹⁷ Kodi cima yathu pa peor sinali yakwanila kwa ife? Koma sitinaziyeleta kucima, Popeza pacimo ija panabwela mulili pa msonkhano wa Yehova. ¹⁸ Naiwenso ufuna kuleka kukonka mulungu pasiku yalelo? Ngati uzaukila nso mungu naiwe lelo, mailo azakalipa na musonkhano bonse wa Israyeli. ¹⁹ Ngati malo yamene ulinayo yabonongeka, mufunika kupitila muziko mwamene cihema ca Yehova cikhala na kuzitengela vinthu pakati kathu. Imwe osabukila mulungu, kapene ife pakumanga guwa yanu malo momanga ya Yehova mulungu. ²⁰ Kodi Akani mwana wa Zera sana phanye cikhulupililo muvinthu viji vinasunguwila mulungu? mukwiyo sunagwele bana ba Israyeli? Uja munthu sanabongeke yekha pa zolakwa zare. ²¹ Pamene mitundu ya A Rubeni, Gadi, na mtundu bogabika pakati wa manase unayankha kuli asogoleli ba mabanja ya Israyeli: ²² Waphamvu, mulungu, Yehova! Waphamvu mulungu, Yehova! - Aziba, lekeni Israyeli azibe! ngati zinali mukuukila kapene mukuphwanya cikhulupililo ca Yehova, Osatisiyako siku iyi. ²³ Pamanga guwa kuzicosa ise teka kukonka imwe Yehova. Ngati timanga guwa cifukwa copeleka nsembe zopseleza, nsembe za ufa, kapene nsembe zamtendele, pamenepo lekan Yehova atilipise. ²⁴ Kapena! tinacita ici kuyopa kuti mu nthawi yobwela ba banu bangakambe kuli bana banthu, 'muli cini imwe kuli Yehova, mulungu wa Israyeli? ²⁵ Popeza Yehova apanga Yolodani malile pakati pathu na imwe. Imwe banthu ba Rubeni na bathu ba Gadi, mulibe vocita na Yehova.' cifukwa cake bana banu angale ngese bana bathu kuleka kulambila Yehova. ²⁶ Cifukwa cake tinakamba, tiyeni manje timange guwa, osati ya nsembe zopseleza kapene ya nsembe zili yonse. ²⁷ Koma kukhala mboni pakati pa ise naiwe, na pakati mibadwa yakusogolo kwathu, kuli tizacita nchitoya Yehova pamenso pake, na nembe zathu zopsele na nsembe zathu na nsembe zathu zamtendele, kuti bana bako sazakamba kuli bana bathu munthawi yobwela," mulibeve mbali mu Yehova." ²⁸ Ndipo tinakamba kuti, ngati izi zifunika kukambiwa kuli ise kapena kuli bana bathu munthawi yobwela, tingakambe kuti," onani! Ici cisanzo caguwa ya Yehova, yamene makolo bathu banapanga, osati ya nsembe zopseleza, kapene nsembe, koma monga mboni pakati kathu naimwe." ²⁹ Zikhale patali naise kuti tiukile Yehova, nalelo kuleka kumukonka iye pakumanga guwa ya nsembe zopseleza na nsembe zaunga, kapenazansembe, mumalo ya guwa ya Yehova mulungu yamene ili pasogolo ya cihema. ³⁰ Pamene phinehasi wansembe na basogoleli ba banthu, bamene, basogoleli ba mabanja ya Israyeli

bamene banali naine, banamva mau yamene banthu ba Rubeni, Gadi na manase banakamba, kuti yanali bwino mumenso. ³¹ Phinehasi mwana wa Eliyaza wansembe anakamba kubanthe ba Rubeni, Gadi, manase," Lelo tiziba kuti Yehova ali pakati pathu, cifukwa simuna phwange cikhulupililo ca Yehova. Manje mwa pulumusa bana ba Israyeli kucoka mumanja ya Yehova. ³² Pamenepo phinehasi mwana wa Eliyaza wansembe nabasogoleli banabwelela kucoka ku A Rubeni na A Gadites, kucoka muziko ya Gileadi, kubwelela muziko ya kenani, kuli bana ba Israyeli, naku bwelesa mau kuli beve. ³³ Mayo yabo yanali ya bwino mumenso ya bana ba Israyeli, Bana ba Israyeli banadaalisa mulungu nakusa kamba ponso zomenya nkondo naba Rubeni na ba Gadites, kuti babonge malo mwamene bana nkhalala. ³⁴ A Rubeni naba Gadites anapasa zina guwa kuti." Mboni popeza banakamba," ni umboni pakati kathi kuti Yehova ni mulungu.

Chapter 23

¹ Patapita masiku yumbili, pamene Yehova anapasa ku pumula kuli Israyeli kucoka kuli adani anali loozanguwka beve, na Yoswa anali bokalamba na zaka zambili. ² Yoswa anaitana bana ba Israyeli, bakulu, na basogoleli bao, na bo weleza bao, na banchita, nakukamba nabeve kuti, "Nakalamba nazaka zapaka." ³ Mwabona vonse vamene Yehova mulungu wako arita ku maziko yonse cifukwa caiwe, popeza ni Yehova mulungu wako wamene akumenyelako. ⁴ Ona! napasa kuli iwe maziko yamene yanasalila ku gonje sewa monga coloba ca mitundu yake, pamozi na maziko yonse yamene nabononga kale, kucokela ku Yolodani kufika kunyanja ikulu kumazulo. ⁵ Yehova mulungu wako azabacosamu. Azabakanka kutali naiwe. Azalanda malo yabo, nakuli iwe uzatenga malo, monga mwamene Yehova mulungu wako analonjezela. ⁶ Cifukwa cake khala olimba, kuti usunge na kucita vonse volembewa mubuku ya cilamulo ca Mose, kupindamukila osati kuzanja yamanja kapena yamanzele. ⁷ Kuti musasakanizane na maiko awa yamene yali pakati pa imwe kapena kutumola mazina ya milungu zabo, kulumbilila pali zeve, kuzilambila, kapena kuzigwadila. ⁸ Koma, mufunika kulamatila kuli Yehova mulungu wanu monga mwame mwacitila kufika lelo. ⁹ Popeza Yehova acosa pamenso yanu maziko yolimba. Kuli imwe kulibe amene akhala akwanisa kuimilila pamene yako kufika lelo. ¹⁰ Munthu umozi azapitikisa bali wanu sauzande, popeza Yehova mulungu wanu, ndiye akumenyelakoni, monga nwamene analonjezela iwe. ¹¹ Muesesa, kuti ukonde Yehova mulungu wako - ¹² Koma ngati wabwelela mbuyo na kulamatila kuli opulumuka ba maziko azasala pakati panu, kapena ngati mwakwatisana nabo kapena mukabwela pamozi nabeve na beve naimwe. ¹³ Pamenepo ziba kuti Yehova mulungu wako azacosanso maziko pakati kanu. Koma, yazakhala msampha na deka kuli imwe, mikwapu kumusana kwanu na minga mumenso yanu, pakana mubonongeke kucoka mumalo yabwino yamene Yehova mulungu wanu akupasani. ¹⁴ Manje nipita munjila ya ziko yonse, ndipo muziba namitima yanu yonse na miyoyo kuti kulibe mav yamozi yakangiwa kucitika ya vinthu vonse yabwino vamene Yehova mulungu wanu alonjeza pali imwe. Ivi vintu vonse vacitikila imwe kulibe nangu cimozi caknga. ¹⁵ Koma monga mwamene mav yaliyonse ya Yehova mulungu analonjeza yakwanilisiwa, kuti Yehova azabwelela pali imwe vonse voipa pakena akubonongeni mumalo aya yabwino yamene Yehova mulungu apasa. ¹⁶ Azacita izi ngati uza phwanya pangano ya Yehova mulungu wako, ywmene anakulamulila iwe kuisunga. Ngati uzayenda kukalambili milingu zina na kuzigwadila, ndipo mkwiyo wa Yehova uzabwela pali imwe, naku bongeka mwamusanga mumalo yabwino yamene akupasa.

Chapter 24

¹ Pamene Yeswa anasonkhaisa mitundu yonse ya Israyeli ku shechem nakuitana bakulu bonse ba Israyeli, basogoleli bao, boweluza, nabanchito, banazibwelesa pamene ya Mulungu. ² Yoswa anakamba kuli banthu bonse," ndiye zamene Yehova akamba, Mulungu wa Israyeli, kukamba kuti makolo yanu kale benze kukhala kusidya ya mumana wa Euphrates - Terah, tate wa Abrahamu natate wa Nahor - na kulambila milungu zao. ³ Koma nunatenga batate bak kubacosa kusidya kwa Euphrates nakubasogolela muziku ya kanani na kumupasa bana bambili kupitila muli mwana wake Isaki. ⁴ Ndipo kwa Isaki ninapa Yakobo na Esau. Ninapasa Esau phili ya ziko yaku Seir kuitenga, koma Yakobo nabana bake banapita ku Egiptu. ⁵ Ninatuma Mose na Anroni, na kulanganga Egiptu namilila, zitapita izo, ninatulosani. ⁶ Ninatulusa makolo yanu mu Egiptu, ndipo unabwela kunyanja. Aigiptu banapepeka beve nama galeta na bamuna bokwela bakavalo kufika ku nyanja yofiila. ⁷ Pamene makolo yanu babalila kuli Yehova, anaika mudima pakati kaiwe na mu Egiptu. Analengesa njanja, ibwele pali beve nakubavwinikila. munaona zamene ninacita mu Egiptu. Pamene munakhala mucipululu nthawi yaitali. ⁸ Ninakuletani kuziko ya Amoni, bamene banakhala kumbali ya Yolodani. Banamenyana naiwe, ninabapasa mumanja yako. Unalandila zio yao, ndipo ninababonga bonse pamenso panu. ⁹ Pamene Balaki umwana wa Zippor, mfumuya moabo, inanyumuka nakumenya Israyeli, Anatuma nakuitana Balamu mwana wa Beor, kutembelela iwe. ¹⁰ Koma sinamvelele kuli Balamu zoona, anakudalisa popeza ninaku pulumusa kukucosa manja mwake. ¹¹ Anatauka pa Yolodani nakufika ku Yeliko. Basogoleli banamenyana naiwe, pamozi na Amori, Aperizi, Akanani, Iti, A Girgashita, A Hivitis, na A Tebusites. Ninakupasani kupambana pali beve nakubaika pansu paulamulilo wanu. ¹² Ninatuma mavu pasogolo panu, yamene yanabacosa na mafumu yabili ya Amoni pamene yako, sizinacitike napanga yako kapene uta yako. ¹³ Ninakupasa malo yamene sunasebenzele na mizinda yamene sunamange, manje ukhalamo. Ukudya vipaso vamumunda na minda ya Olivi yamene sinashange! ¹⁴ Manje yopa Yehova nakulambila iye na ulemu onse na kukhulupilika: bononga milungu imene makolo banalambila kusidya ya Euphrate, na mu Egiptu, na Kulambila Yehova. ¹⁵ Ngati zibuneka zoipa mumenso yako kuti ulambila Yehova, zisankhile weka lelo wamene uzatumikila, kapena milungu ya makolo yanalambiliwa kusidya ya Euphrates, kapena milungu za Amori, mumalo mwabo mwamene ukhala. Koma kwaine na nyumba yanga, tizalambila Yehova. ¹⁶ Banthu banayankha nakukamba kuti," sitingaibale Yehova kutumikila milungu zina. ¹⁷ Popeza ni Yehova mulungu wathu anatikweza ku tiosa miziko ya Egiptu, kuciosa munyumba yaukapolo, amene anacita zizindikilo zikulu mumeneso mwathu, anatisunga munjila zonse zamene tinayenda, na pamaziko yonse tina pitamo. ¹⁸ Ndipo Yehova anacokapo pamenso pabanthu bonse, kufikilako ba Amori banakhala mu zio. Cifukwa cake naife tinalambila Yehova, popeza ni mulungu wathu. ¹⁹ Koma Yoswa anakamba kuli banthu kuti," simungatumikila Yehova, popeza nimulungu boyela; Ni mulungu wa nsanje,' sazakhulukilila zolakwa zanu na macimo yanu. ²⁰ Ngati mwamusiya Yehova nakulambila milungu zina, pamene azatembunuka nakcita zoipa pali imwe. Azakusilizani, pambuyo pokucitilani zabwino. ²¹ Koma banthu banakamba kuli Yoswa," Iyai, tizalambila Yehova. ²² Pamenepo Yoswa anakamba kuli banthu," ndimwe mboni zaimwe weka kuti mwasankha Yehova, kumulambila iye," Banakamba," Ndife mboni." ²³ Manje cosani milungu zacilendo zamene muli nazo, penyesani mitima yanu kuli Yehova, Mulungu wa Israyeli." ²⁴ Banthu banakamba kuli Yoswa," tizalambila Yehova mulungu wathu tizamvela mau aya." ²⁵ Yoswa anapanga cipangano nabantu siku ija. Anaika zinenelo na malamuno mu shechemu. ²⁶ Yoswa analemba mau aya mubuku yacilamulo ca mulungu. Anatenga mwana ukulu na kuika pakati ka mtengo wa nthundu wamene unali pafupi malo yopa tulika ya Yehova. ²⁷ Yoswa anati kuli banthu bonse," ona, uyu mwala uzkhala umboni wotisusa. Tamva mau yonse Yehova wakamba kuli ife. cifukwa cake izakhala mboni yokosusa, ngati uzafuma kukana mulungu wako. ²⁸ Pamenepo Yoswa anabuza banthu kuti bayende, alibonse kucoloba cake. ²⁹ Zitapita izi Yoswa mwana wa Nuni, mutumiki wa Yehova, anamwalila, nazaka 110. ³⁰ Banamushika mumalile yacoloba cake, pa Timnath Serah, yamene ili muphili yaziko ya Eflemu, ku mpoto kwaphili ya Gaash. ³¹ Israyeli analambila Yehova masiku yonse ya Yoswa, na masiku yonse ya bakulu banakhala zaka kupamba na Yoswa, baja banabona vose yamene Yehova anacita kwa Israyeli. ³² Mafupa ya Yosefe, yamene ba ba Israyeli babaleta kucosa mu Egiptu - banaya shika pa shechem, mumalo yamunda mwamene Yakobo anagula kuti bana ba Hamor, tate wa shechem. Anaigula pa wanu handiledi ya siliva, ndipo ina khala coloba cabana ba Yosefe. ³³ Eliyaza mwana wa Aaroni anamwalila nayeve. Banamushikila pa Gibeah, muzinda wa phinehasa mwana wake, yamene yenze inapasiwa kuli yeve. Inali muphili yaziko ya Eflemu.

Judges

Chapter 1

¹ Pamene inapita imfa ya Yoswa, bantu ba Israeli banafunsa Yehova, kuti, "wamene azayambilila kutimenyela ba Kenani nindani, kubamenyela beve?" ² Yehova anakamba kuti, "Yuda azamenyela. Onani, nabapasa ulamulilo pali aya malo." ³ Bamuna ba Yuda banakamba kuti kuli bamuna ba Simiyoni, babululu bao, "bwelani paozi na ife mu ziko yatu yamene inapasiwa kul ife kuti timenyele ba Kanani. Tizacita comozi-mozi kupita na imwe ku malo yamene munapasiwa." Apo mtundu wa Simiyoni unayenda na beve. ⁴ Bamuna ba mu Yuda banamenya, na Yehova anabasa kupambana pali ba Kenani na ba Perize. Banapaya bali teni sauzande pa Bezeki. ⁵ Banapeza Adoni-Bezeki pa Bezeki, nakumenyana na eve ku pambana ba Kenani na ba Perize. ⁶ Koma Adoni-Beze anataba, ndipo banmukonka nakumugwila, banamujuba vikumo vakumanja na vikumo vake vikulu vakumendo. ⁷ Adoni-Bezeki anamba kuti, "Mafumu sevente, bamene banajubiwa vikumo va kumanja na vikumo vao vikulu vakumendo, banika pamozi vakudya munyansi ya tebo yanga. Mwamene ninacitila, na Mulungu wanicitila futi cimozi-mozi." Banamuleta ku Yerusalemu, nakufa kwamene kuja. ⁸ Bamuna ba mu Yuda manamenyela mzinda wa Yerusalemu nakuutenga. Banamenyela na kotela kwa mupeni na kuuyasha mulilo munznda. ⁹ Kucoka apo, bamuna ba Yuda banseluka nakuyendo menyana na ba Kenani bamene benzonkala mu malupili, ku Nagev, na kumalo yonkazikika. ¹⁰ Yuda anayenda futi kuli ba Kenani benzonkala ku Hebroni (zina ya Hebroni kudala yenze Kiriati Ariba), banagonjesa Sesai, Ahimani, na Talimai. ¹¹ Kucoka uko bamuna ba Yuda banayenda kumenyana na nzika zaku Debiri (zina ya Dibiri kudala yenze Kiriati Seferi). ¹² Kalebu anakamba kuti, "aliyense wamene azakamenya Kiriati seferi nakutinga, nizamupasaa Akisa, mwana wanga mukazi, kuti ankale mkazi wake." ¹³ Otiniyeli, mwana mwamuna wa Kenazi (mufana wake wa Kalebu) anamugwila Dibiri, Kalebu anamupasa Akisa, mwana wake mukazi, kuti ankale mukazi wake. ¹⁴ Manje Akisa anabwela kuli Otinieli, nakumuza kuti auze batate bake kuti amupase munda. Pamene enzeli kuseluka pa bulu, Kalebu anamufunsa, "ufuna nikucitile cani?" ¹⁵ anakamba kuti kuli eve, "nipaseni daliso. Pakuti mwanipasa malo kalu Nagev, munipase futi visime va manzi." Apo Kalebu anamupasa visime vakumwamba na visime va pansi. ¹⁶ Bana obadwa kumbuyo ba apongozi bake ba Mose ma Kenite bana kwela kucokela ku mzinda wa Kanjeza na bantu ba Yuda, kupita mu cipululu ca Yuda, camene cili ku Nagev, kuyenda kunkala na bantu ba ¹⁷ Yuda pafupi na Aradi. Bamuna ba Yuda banayenda na bamuna ba Simeoni babululu bao nakumenya ba Kenani bamene bankala ku Zefati nakuiongelatu. Zina ya muzinda wenze kuitaniwa kuti Horima. ¹⁸ Bantu ba Yuda banatenga futi Gaza na malo oizungulila, Ashkeloni na malo oizungulila, na Ekroni na malo oizungulila. ¹⁹ Yehova enze na bantu ba Yuda ndipo banatenga ziko yakumalupili, koma sibanapishe nzika zaku cigwa cifukwa benze na akavalo ba nsimbi. ²⁰ Hebuloni wenze unapasiwa kuli Kalebu (monga mwamene Mose anakambila), nakuti muja anapishamo bana batatu ba Anaki. ²¹ Koma bantu ba Benjamini sibanapishe ma Jebusites bamene benzonkala mu Yerusalemu. na ma Jebusites bankala na bantu ba Benjamini mpakana lelo. ²² Nyumba ya Yosefe inakonzekela kumenyana na Beteli, apo Mulungu enzeli na beve. ²³ Banatumiza bamuna kuyendo fufuza ku Beteli (Muzinda wamene kudala benze kuuitana Luzi). ²⁴ Bofufuza banaona mwamuna acokela mumuzinda, ndipo banamba kuti kuli eve, "tilangize, tapapata, mwamene tingangele mumzinda, nakuti tizakumvelela cifundo." ²⁵ Aanabalangiza njila yongenela mumzinda, pamene apo banamenya mzinda na kotela kwa mupeni, koma banamuleka mwamuna uja na banja yake kuyenda. ²⁶ Apo mwamuna anayenda ku malo ya Ahiti nakumanga muzinda nakuuitana kuti Luzi, yamene ni zina yake na manje. ²⁷ Bantu ba Manase sibanapishe bantu bonkala mu mizinda ya Beti Sani na minzi yake, kapena Tanaki na minzi yake, kapena baja bonkala mu Dori na minzi yake, kapena baja bonkala Ibleamu na minzi yake, kapena baja bonkala mu Megido na minzi yake, cifukwa ba Kenani benze bofunisisa kunkala mu malo yaja. ²⁸ Pamene Israeli anankala wampamvu, anakakamiza ba Kenani kubasenzela na nchito yolimba, koma sibanabapishletu. ²⁹ Efraimu sanapishe Bakani bamene benzonkala ku Gezeri, telo bakanani banapiliza kunkala ku Gezeri pakati pao. ³⁰ Zebuluni sanapishe bantu bonkala kuKitroni, kapena bantu bonkala k Nahaloli, apo ba Kanani banapitiliza kunkala nao, koma Zebuluni anakakamiza Kenani kubasenzela na nchito yolimba. ³¹ Aseri sanapishe bantu bonkala ku Ako, kapena bantu bonkala ku Sidoni, kapena baja bonkala ku Akalabu, kapena Akisibu, kapena Heliba, kapena Afiki, kapena Rehobo. ³² Telo mutundu wa Aseri unankala pamozi na ba Kanani (baja benzonkala mu malo), cifukwa sanabapishe. ³³ Mutundu wa Nafitali sanapishe baja bonkala mu Beti Semesi, kapena baja bonkala mu Beti Anati. Telo mutundu wa Nafitali unankala pamozi na ba Kanani (baja bantu benzeli kunkala mu malo). Motelo, nzika za ku Beti Semesi na Beti Anati banakakamiziwa kumugwilila nchito yolimba Nafitali. ³⁴ Ba Amori anakakamiza mutundu wa Dani kunkhala mu ziko yakumalupili, kosabavomeleza kuseluka ku cigwa. ³⁵ Telo ba Amori banakala ku lupili ya Heresi, mu Ajaloni, na mu Saalibimu, koma nyumba ya

asilikali ya mphamvu ya Yosefe inabagonjesa, nakubakakamiza kubasenzela nchito yolimba.³⁶ Malile ya Amori inacokelaku lupili ya Akrabimu ku Sela kufika ku ziko yaku malupili.

Chapter 2

¹ Mu ngelo wa Yehova anakawela kucoka ku Giliga kupita ku Bokimu, na kukamba kuti, "ninakucosa iwe mu Egipto, nakukuleta ku malo yamene ninalumbila kupasa makolo bako. Ninakamba kuti, 'sinapwanya pangano yanga na iwe.' ² Siufanikila kupanga pangano na baja bamene bankala mu malo yano. Ufanikila kupwanya ma guwa yao.' Koma sunamvele mau yanga. Nicani ici camene wacita? ³ Telo manje nikuti, 'sinizapisha ba Kanani pamenso pako, koma banzakala minga mu mbali mwanu, na milungu yao izankala misampha kuli imwe.'" ⁴ Pamene mungelo wa Yehova anakamba mau aba kuli bana ba Israeli, bantu banakuwa na kulila. ⁵ Banaitana malo ao Bokimu. Pamene paja banapeleka nsembe ku Yehova. ⁶ Manje pamene Yoswa anabaleka bantu kuti bayende, bantu ba Israeli banayenda kumalo kwamene banapasiwa, kutenga coloba pa malo yao. ⁷ Bantu bantumikila Yehova mu ntawi ya moyo wa Yoswa na bakulu bakulu banasala pamene Yoswa anafa, baja bamene banona vikulu vamene Yehova anacitila ba Israeli. ⁸ Yoswa mwana wa Nuni mtumiki wa Yehova, anafa na zaka 110. ⁹ Banaika tupi yake mu malile ya malo yamene enze anapasiwa mu Timinati Heresi, mu ziko ya kumalupili ya Efraimu, kumpoto kwa lupili ya Gasi. ¹⁰ Mubadwo wonse unasonkanisiwa kuikiwa kwa batate bao. mubadwo winangu unakula kucoka beve wamene sunazibe Yehova kapena vamene anacitila Israeli. ¹¹ Bantu ba Israeli banacita vintu voipa pamenso pa Yehova nakutumikila abaala. ¹² Banacoka kuli Yehova, Mulungu wa makolo bao, wamene anabacosa mu ziko ya Egipto. Nakukonka milungu inangu, milungu yamene yaja ya bantu bamene benzeli kunkala nao, nakubagwadila beve. Banausha ukali wa Yehova cifukwa ¹³ banacoka kuli Yehova nakutumila baala na asitaroti. ¹⁴ Ukali mwa Yehova unashoka Israeli, na kubapeleka ku bantu benangu bamene banabela vintu vao. Anabagulisa monga akapolo bamene bagwiliwa na mpamvu za adani bao obazungulila, mwakuti sibanakwanise kuziteteza kuli badani bao. ¹⁵ Pali ponse pamene Israeli ayenda ku nkondo, kwanja ya Yehova inbakalipila na kubagonjesa, monga mwamene alumbila kuli beve na kuti banavutisiwa maningi. ¹⁶ Pamene apo Yehova anyamula Oweruza, wamene anabapulumusa mu manja ya baja benzeli lkubabela vintu vao. ¹⁷ Koma sibana mvele oweruza. Benze osakulupilika kuli Yehova nakuzipeleka monga mahule ku milungu inangu nakuyapembeza. Banayendisa kucoka mu mbali mwamene makolo bao benzeli kunkalila.-baja bamene banaknka malamulo ba yehova-koma beve beka sibanacite. ¹⁸ Pamene Yehova anabanyamulila oweruza, Yehova anatanidiza oweruza nakubapulumusa ku adani bao mu masiku yonse yamene oweruza anankala. Yehova anabacitila cifundo pamene badandaula cifukwa ca baja bamene babapondeleza nakubavutisa. ¹⁹ Koma pamene oweruza anafa, banali kucokako nakucita vintu voipa maningi kucila vamene banaccita batate bao. banali kukonka milngu inangu na kuipembeza. Banakana kuleka voipa vao vilivonse vamene banali kucita kapena njila zao za ntota. ²⁰ Ukali wa Yehova unashoka Israeli; anakamba kuti, "Cifukwa ziko iyi yapwanya malamulo ya cipangano camene nenze ninaika pali makolo bao- cifukwa sibanamvele mau banga- ²¹ kucoka manje, sinizacosa, ziko iliyonse yamene Yoswa anasiya pamene anafa. ²² Nizacita ici kuti niyese Israeli, kuti bazasunga kepana sibazasunga njila za yehova nakuyendamo, monga batate bao banaisunga." ²³ Nicifukwa cake Yehova anayaleka maziko ayo nakusabacosamo mofulumiza nakubapeleka mu manja ya Yoswa.

Chapter 3

¹ Tsopano Boazi anakwera kuchipata ndipo anakhala pansi pomwepo. Posakhalitsa, wachibale wapafupi amene Boazi ananena za iye anadza. Bowazi anati kwa iye, "Bwenzi langa, bweru udzakhale pansi apa." Munthuyo anabwera nakhala pansi. ² Kenako Boazi anatenga amuna khumi mwa akulu a mzindawo nati, "Khalani pansi apa." Koteri iwo anakhala pansi. ³ Bowazi anati kwa wachibale wapafupi uja, "Naomi, amene wabwera kuchokera kudziko la Mowabu, akugulitsa malo amene anali a Elimeleki mchimwene wathu. ⁴ Ndinaganiza zokukuwuzwa ndikuti, Ugule pamaso pa anthu amene ndakhala pano, pamaso pa akulu a anthu anga. ' Ngati ukufuna kuiwombola, uwombole. Koma ngati simukufuna kuiwombola, ndiuzeni kuti ndidziwe, chifukwa palibe wina amene angaiwombole kupatula iwe, ndipo ine ndiri pambuyo pako. " Kenako munthu winayo anati, "Ndikuwombola." ⁵ Ndipo Boazi anati, "Tsiku lomwe udzagula mundawo kwa Naomi, utengere Rute Mmoabu, mkazi wamasiye wa munthu wakufa, kuti ukwezeke dzina la womwalirayo pa cholowa chake." ⁶ Kenako wachibale wapafupi uja anati, "Sindingathe kuziwombola ndekha popanda kuwononga cholowa changa. Utege ufulu wanga woti wombole wekha, chifukwa sindingathe kuuwombola." ⁷ Tsopano uwu unali mwambo wawo mu Israeli wakale wokhudza kuwombola ndi kusinthanitsa katundu. Kuti atsimikizire zinthu zonse, munthu adavula nsapato yake ndikupereka kwa mnzake; Umu ndi momwe ankapangira mapangano mu Israeli. ⁸ Wachibale wapafupiyo adati kwa Boazi, "Ugule iwe," ndipo adavula nsapato yake ⁹ Ndipo Bowazi anati kwa akulu ndi anthu onse, Inu ndinu mboni lero kuti ndagula zonse za Elimeleki, ndi zonse za Kilioni ndi Maloni m'manja a Naomi. ¹⁰ Komanso Rute mkazi wachimoabu, mkazi wa Maloni, ndatenga mkazi wanga, kuti ndikweze dzina la wakufayo pa cholowa chake, kuti dzina lake lisachotsedwe pakati pa abale ake ndi pa chipata cha kwawo: Lero ndinu mboni! " ¹¹ Anthu onse amene anali pachipata ndi akulu anati, "Ndife mboni. Yehova achite kuti mkazi amene wabwera m'nyumba mwako akhale ngati Rakele ndi Leya, omanga nyumba ya Israeli; ndipo zikuyendere bwino mu Efurata. ¹² nyumba yako ikhale ngati nyumba ya Perezi, amene Tamara anambalira Yuda, mwa mbewu imene Yehova adzakupatsa pamodzi ndi mtsikana uyu. ¹³ Ntheura Bowazi wakatora Rute, ndipo wakawa muwoli wake. Ndipo analowa kwa iye, ndipo Yehova anatsegula pakati, ndipo anabala mwana wamwamuna. ¹⁴ Akaziwo anati kwa Naomi, "Adalitsike Yehova amene sanakusiye lero wopanda wachibale wapafupi, mwana uyu. Dzina lake litchuke mu ¹⁵ Israeli. Akhale kwa inu wobwezeretsa moyo ndi wosamalira ukalamba wanu, chifukwa mpongozi wako amene amakukonda, amene wakuposa ana amuna asanu ndi awiri wamubereka. ¹⁶ Naomi anatenga mwanayo, namugoneka pachifuwa pake, ndi kumusamalira. ¹⁷ Akazi oyandikana naye adamutcha dzina, nati, "Kwa Naomi kwabadwa mwana wamwamuna." Anamutcha dzina lakuti Obedi. Iye anabereka Jese, amene anabereka Davide. ¹⁸ Ana a Perezi anali awa: Perezi anabereka Hezironi, ¹⁹ Hezironi anabereka Ramu, Ramu anabereka Aminadabu, ²⁰ Aminadabu anabereka Nasoni, Nasoni anabereka Salimoni, ²¹ Salimoni anabereka Boazi, Boazi anabereka Obedi, ²² Obedi anabereka Jese, Yese anabereka Davide.

1 Samuel

Chapter 1

¹ Kunali mwamuna winangu waku Ramathayimu wa mutundu wama Zufayite, wa ziko yakumutunda wa Efuramu; zina yake anali Elukana mwana wa Jerohamu mwana mwamuna wa Eliwu mwana wa Towu mwana wa Zufu, wakumutundu wa chimasulidwe chamauli na Ramathayimu Zofayimu, koma chimaziwika kuti Zofayimu iyimilila maningi malo mwamene mbadwo unachokela kwamene Zufu anaukhala. ² Anali na azikazi abili; zina ya woyamba anali Hanna, ndipo zina ya wachiwili inali Peninna. Peninna anali na wana, koma Hanna analibe loko mumozi. ³ Uyu munthu anali kuchokela ku tawuni ya kwao chaka na chaka nakubwela ku shilo kupembeza nakupeleka nsembe kwa Ambuye Yehova. Wana wamuna abili wa Eli, Hofini na Finiyasi, ansembe wa Yehova, anali kwameme. ⁴ Siku ikafika yakuti Elukana apeleke nsembe chaka chili chonse, nthawi zonse zigawo za nyama kuli Peninna mkazi wake, na kuli wonse wana wake wamuna nawakazi. ⁵ Koma kuli Hanna nthawizonse anali kupasa vambili maningi, pakuti anamukonda Hanna, mimba yake. ⁶ Pofuna kumuyamba, mkakazi mzake anali kumukalipisa kabili kabili, chifukwa Yehova anamuvala mimba yake. ⁷ Apo chake na chaka, akayenda ku nyumba ya Yehova na banja yako, mdani wake mpaka amukalipise. Nchifukwa chake anali kulilalila nakasadya kanthu. ⁸ Elukana mwamuna wake nthawi zonse anali kuti kwa yeve, "Hanna, ulila chani? Ulekelanji kudya? Mtima wako ukunyililanj? Kodi ine sini pambana wana wamuna bali teu?" ⁹

Chinachitikapo siku inangu mwa imozi mwa aya masiku , Hanna ananyamuka watasiliza kudya nakumwa ku Shilo . Apa Eli wansembe enze anaukhala pa mupando wake wapa fupi na polowela mu tempile ya Yehova. ¹⁰ Enze anavutika kuchokela pansu pa mutima wake ; anapemphela kwa Yehova na kulila mokuwa mwaukali maningi. ¹¹ Anapanga chipangano kuwana kuti , " Yehova wa makawu , ngati muzayanganila kuvutika kwa kapolo wanu nakumukambukila mumutima mwanu , nakusamuyiwala kapolo wan , koma mumupase kapolo wanu mwana mwamuna , pasogolo pake ine nizamupasa kwa Yehova masiku onse amoyo wake ndipa kulibe kaleza kazaka kumyako mutu wake". ¹² Pamene anapitiliza kupembhera kwa Yehova , Eli anali kumuyang'ana pakamwa . ¹³ Hanna anali kukambila mumutima mwake . Milomo yake inali kunyang'anya koma mau yake siyanali kunveka . Apo Eli anaganiza kuti Hanna anali wokolewa. ¹⁴ Eli anamuwuzwa kuti , " Uzankhala wokolewa mpaka liti ? uwuleke mowa wako. ¹⁵ Hanna anayankha , " Iyayi abusa wanga, ndine muzimayi wa muzimu wokwinyilila . Sininamweko wayini loko munkhoyo ukali , koma nankhala nithila moyo wanga kwa Yehova. ¹⁶ Musamuganizile kapolo wanu kunkhala muzimayi wamusewanya ; nankhala nikamba kuchokela wuku khuziwa maningi nakavunduliwa". ¹⁷ Apo Eli anayankha nakukamba kuti , " Yenda mwanitendele ; Mulungu wa Isirayeli a funika akupase chamene wamupempha." ¹⁸ Anayankha kuti , " Lekani kapolo wanu apeze chifundo mumanso mwanu . " Apo muzimayi anayenda kwawo na kudya ; nkhope yake siyinawoneke futi yokwiya. ¹⁹ Anauka m'mawamawa maningi nakupembeza Yehova , ndipo wanabwelela futi kunyumba kwao ku Roma . Elukana anagonana na mukazi wake , ndipo Mulungu anamukumbukila yeve. ²⁰ Pamene nthawi inakwanila , Hanna anankhala namimba nakubala mwana mwamuna . Anamuyitana zina yako Samweli , kutanthauza kuti , " Chifukwa ninamumphepha kwa Mulungu." ²¹ Nafuti , Elukana na wamunyiimba yake wonse wanayenda kukapeleka kwa Yehova nsembe ya chaka na chaka nakukalipila chilayo chake . ²² Koma Hanna sanayende , anati kuli mwamuna wake , "Sinizayenda mpaka mwana akaleke kunyonkha ; ndiye pamene nizamuleta , kuti akaonekele pamenso pa Yehova nakunkhala kwamene kuja kwamuyaya." ²³ Elukana mwamuna wake anakamba kuti kuli yeve , " Uchite chamene chikuwonekela bwino kwa iwe. Yembekeza mpaka ukamulumule ; chabe , leka Mulungu asimikize mau yake ." Apo muzimayi uja anasala nakulela mwana wake mpaka kumulesakunyonkha. ²⁴ Atamulesa kunyonkha , anamutenga pamozi na ng'ombe imuna yazaka zitatu, mpiwo umozi wa ufa , na botolo imozi ya wayini , nakumuleta kunyumba ya Yehova ku Shilo . Apa mwana enze akali m'ng'ono. ²⁵ Anapaya ija ng'ombe imuna , nakumuleta uja mwana kuli Eli. ²⁶ Anati , " Oh , Abusa wanga ! Mukali na moyo , Abusa wanga , ndiwe mkazi uja wamene anayimilila pamene pano kupemphela kwa Yehova . ²⁷ Ninapempha uyu mwana ndipo Yehova ananipasa yankho ya dandaulo yanga yamene ninamupempha. ²⁸ Namupasa kwa Yehova , makoinga ali mamoyo niwobwelekewa kwa Mulungu ." Chokonkhalo anapembeza Yehova pamene apo .

Chapter 2

¹ Hanna anapemphela ati , " Mtima wanga ukondwela muli Yehova . Nyanga yanga ikwezedwa muli Yehova kamwa kanga kazikweza kupambana wadaui wanga , chifuka nilinachikondwelelo mu chipulumuso chawu. ² Kulibe wolungana monga Yehova , chifuka kulibe winangu kupatulapo imwe ; kulibe mwala monga Mulugu wathu. ³ Osazikweza futi momeka; musachoke nthota kufuma mukamwa mwanu , pakuti yehova ni Mulungu woziwa; niyeve awapiwa zichitidwe. ⁴ Uta wa wanthu wamphavu umatyoka koma waja ozezelakela kwa Mulungu amavala mphavu monga ni beluti. ⁵ Waja wenze wokuta wayenda kungena ganyu yo fola buledi ; waja wenze nanjala waleka kunkhala wanjala. Olo wosabala abeleka wana seveni koma nikazi wamene ali na bana wmbilili avutika kosapeza thandizo. ⁶ Yehova amapaya nakuwukisha ku umoyo . Amangenesa pansi mu manda naku ukisha. ⁷ Yehova amapanga wanthu wenangu wosauka ndipo wenangu wolemela . Amachepesa , koma amanyamula futi. ⁸ Amanyamula osauka kuwachosa mudothi . Amanyamula osowekela kuchoka pa culu cha milota kuwalengesa wankhala pamozi na wana wama fumu nakupyanika pa chipuna cha ulemu .Pakuti vipilala vaziko yapansi niva Yehova ndipo anankhazika chalo pali veve. ⁹ Azaleselela mendo ya banthu wake wokhulipilika . Koma wamaganizidwe woyipa azawayika chete mamudima , pakuti kulibe aza pambana na mphanvu. ¹⁰ Waja wamene wavutana na Yehova wazaphwanyiswa mutumagawo; aza waulumila mwaukali mowasusha kuchokela kumwamba . Yehova azapasa mphanvu kuli mfumu yake nakukweza nyanga ya ozezedwa wake. ¹¹ Ndipo Elukana anayenda ku Rama kunyumba kwake . Uja mwana anali kutamikila yehova mu menso mwa Eli wausembe . ¹² Koma wana wamuna wa Eli benze wachabe chabe . Sibana muziwe Yehova . ¹³ Mwambo wa wausembe na banthu unali wakuti munthu aliyense akapeleka nsembe , mtumiki wawansembe analikubwela na foloko yavolasila vitatu m'mauja mwake , pamene nyama yenze ikali kubila. ¹⁴ Enzekuyidinikizila mu pani , olo ketulo , olo muchi shomeka olo mupoto Zonse zamene zinachosewa panja na foloko wansembe znalikutenga nizake .Anachita sochabe ku Shilo na wonse waku Israeli wamene wanali kubwelako. ¹⁵ Kuyipikilako kwake , akalibe kushoka mafuta , nitumiki wothandiza wansembe anali kubwela , nakukamba kuli munthu wamene enzopeleka nsembe , " Pasa nyama nyama yobilisa yochokela kuli iwe , koma chabe ibishi." ¹⁶ Ngati uja munthu anamuyankha kuti , " Wafunika kushoka mafuta poyamba , ndipo pambuyo pake utenge vambili mwamene ufunila." Apo anali kuyankha kuti " Iyai , uzayipeleke manje apa ; ngati iyai, niyitenga mwachikakamizo." ¹⁷ Chimo ya awa wanyamata inali ikulu maningi pamenso pa Yehova , Ndawa ananyozela chopeleka cha Yehova. ¹⁸ Koma Samweli anatumikila Yehova monga mwana woala efodi yanyula yatelela. ¹⁹ Amai wake anali kumupangila kamukhanjo kang'ono nakumubwelesela chaka na chaka , pamene analikubwela na wamuna wake kupeleke nsembe ya chaka nachaka. ²⁰ Eli anali kudalisa Elukana na mukazi wake kuti , " Mulungu akudalise na bana wambili kupitila muli uyu mukazi chifukwa cha pemphelo yamene ana peleka kwa Yehova ." Wakasiliza banali kubwelela kunyumba kwao. ²¹ Yehova anamuthandiza futi Hanna , ndipo anankhala futi na mimba . Anabala bana bamuna watatu na bana wakazi batatu. Apo munthawi iyi naye mwana Samweli anakulila mumenso mwa Mulungu . ²² Apo manje ninshi Eli anali atakalamba maningi , anamvela zonse zamene wana wake wamuna wanali kuchita ku Israeli yonse , na mwamene analikugonelana polowela mu tenti yamusoukhano. ²³ Anati kwa weve , " Muchiti lanji vinthu vamutundu uyu?" Pakuti nimvela zidutidwe zana zoyipa zonse kuli aba wanthu. ²⁴ Iyayi , wana wanga ; ndawa silipoti yabwino yamene nimamvela . Muwalengesa aba wanthu wa Yehova wasamvele Mulungu. ²⁵ Ngati munthu mumozi wachimwila muuzake , Mulungu azamuweluzi . Koma ngati munthu achimwila Yehova ndani azamukambilako? " Koma siwanamvele mau yabatate bawo ndaba Yehova ana anachipanga kuti awapaye . ²⁶ Mwana Samweli anakula , nakuonjezeleka kukondewa na Mulungu na banthu. ²⁷ Apo munthu wa Mulungu anabwela kwa Eli nakunena kuti kuli yeve, "Yehova akuti ' kedi ine sininaziulule neka kubanja ya atate wako pamene anali ku Egiptito mu ukapolo ku akunyumba ya Pharawo?" ²⁸ Ninamusankha kuchokela pa mikoka yonse ya Israeli kuti aukhale wausembe wanga , kuti azikwela kuguwa yanga , kuti azishoka usembe zofwaiza , kuti azivala efodi pamenso panga .Ninapasa kwa akunyumba kwa atate bako zopeleka zouse za banthu wa Israeli zopangiwa na mulilo. ²⁹ Chifukwa , manje , chamene usewanyila nsembe na zopeleka zamene nifuna mumato mwamene ninkhala ? chifukwa ulemekeza bana bako kuchila pali ine pozidyesa mpaka mwaziyinisha mweka na zopeleka zabwino maningi za wanthu baku Israeli?' ³⁰ Pakuti Yehova Mulungu wa Israeli , akuti , ' Nilonjeza kuti akunyumba yako na banja ya tate bako afunika kuyenda pamaso panga kwamuyaya koma manje Yehova akuti , ' Nchapatali kwa ine kuti nichite ichi , pakuti nizalemekeza waja wamene wanilemekeza , koma waja wamene wanisula sinizaiwala loko pang'ano zochita zao. ³¹ Ona , masiku ya zabwela pamene nizajuwa mphanvu zako na mphanvu za akunyumba ya atate bako . ³² Uzaona kusoweka ntendele mumalo mwamene ninkhala . Angakhale ubwino uzapasiwa kwa Israeli , sikuzakankhalapo futi munthu wokota mubanja mwako. ³³ Aliyonse wa imwe wamene sinina muchoseko kuguwa

yanga , niza chitisa menso yako kuti yasazi wona, ndipo nizachitisa kukwinyilila mumutima mwako , ndipo aliyense wa wobadwa wako wazafa. ³⁴ Apo ichi ndiye chizankhala chozibilako chamene chizabwela pa bana wako babili , pali Hofini na Finiyesi wonse wabili wazafa siku yimozi. ³⁵ Nizazinyamulila neka wansembe wanga wokhulapilika wamene azachita vilimu mutima mwanga na mumoyo wanga . Nizamu mangila nyumba yosakayikisa; ndipo azayenda pamenso pa mfumu yanga yozozedwa kwa muyaya. ³⁶ Aliyense wamene azakasalako mu banja yako azakabwela nakumugwalila , kumupempha ndalama na buledi , na kukamba kuti , "Napapata nitumenikoni pa imozi mwa nchito yawunsembe pakuti ningadyeko kanyenyekwa ka buledi."

Chapter 3

¹ Mnyamata Samweli anatumikila Yehova mokonkhala usogoleli wa wa Eli . Mau a Mulungu anali osowekela ayo masiku ; Mensomphenya ya aneweri siyanali kubwera pafupi pafupi . ² Panthawi iyo , pamene Eli , wamene menso yake yanayamba kuchita chimbuwila kivakuti senzoyangana bwino , anali gone mu bedi yako . ³ Nyale ya Mulungu yenze ikalibe kuzima , na Samweli analigone mutempile ya Yehova , pamalo pamene panali chombo chachipangano cha Mulungu . ⁴ Yehova anamuyitana Samweli , wamene anayankha kuti , "Nili pano." ⁵ Samweli anathawira kwa Eli nati , "Nili pano , kamba kuti mwanayitana ." Eli anati , "Sininakuyitane; kagone futi ." Apo Samweli anayenda nakugona pansi . ⁶ Yehova anayitana futi , "Samweli " Nafuti Samweli anauka nakuyenda kukamba kuli Eli kuti . "Nili pano pakuti imwe mwaniyitana ." Eli anayankha , "Sininakuyitane , mwana wanga ; gona pansi futi." ⁷ Apa Samweli anali akalibe kuziwa mochitila na Yehova , futi kwenze kukalibe kuwululikako uthenga uli wense wochoka kwa Mulungu kuli yeve . ⁸ Mulungu anayitana Samweli futi Samweli kachitatu . Nafuti Samweli anauka nakuyenda kuli Eli ali , "Nilipano , kawili mwaniyitana ." Apo Eli anaziwa kuti Yehova ndiye enze ayitana mnyamata . ⁹ Ndipo Eli anati kwa Samweli , " Yenda ugone pansi futi ; akakuyitana futi ukambe kuti , 'Kambani , Yehova , pakuti kapolo wanu ali kumvela : 'Apo Samweli anayenda ku gona futi pansi pamalo pake. ¹⁰ Yehova anabwela nakuyimilila ;anayitana monga panthawi zoyambilila , "Samweli Samweli ." Apo Samweli anati , " Kambani , chifukwa kapolo wanu ali kumvelelela." ¹¹ Yehova anati kwa Samweli , "Ona , nasala pang'ono kuchita chinthu mu Israeli chamene kwatu iliyonse ya aliyense wamene azachimvela izalila mwa chongo. ¹² Pasiku iyi nizachita mosusana na Eli na wamunyumba mwake vonse vamene ninakamba , kuchokela poyamba mpaka manje. ¹³ Ninamuwuzi kuti nasala pang'ono kuweluzi nyumba yake kuweluzilatu chimo yamene anali kuziwilatu , chifukwa wonse anyamata wake anaziletela weka tembelelo koma yeve sanawalese. ¹⁴ Chifukwa cha ichi nalapila panyumba ya Eli kuti machimo yabanja yake siyizaleseleleka olo na nsembe kapena chopeleka . " ¹⁵ Samweli anagona pansi mpaka m'mawa; ndipo ana segula viseko va nyumba ya Yehova . Koma Samweli anayopa kuwuzi Eli za masomphenya yaja. ¹⁶ Ndipo Eli anayitana Samweli na kunena kuti , " Samweli , mwana wanga ." Samweli anati "Nili pano." ¹⁷ Anati akuwuzi mau yabwanji ? Chonde asochibisa kuli ine . Mulungu akuchitile ichi , ndipo nakuwonjeselapo maningi, ngotanakukambisa iwe." ¹⁸ Samweli anamuwuzi vonse ; palibe chamene anabisapo . Eli anati , " Ni Mulungu . Mulekeni achite chamene chimuonekela bwino kwa yeve ." ¹⁹ Samweli anakula ndipo Mulungu anali naye , ndipo sanalole kuti olo imozi mwa mau ake auneneli agwele padela . ²⁰ Israeli yonse kuyumbila pa Dami mpaka ku biyashiba anaziwa kuti samweli anasankhiwa kunkhala m' neneli wa Yehova . ²¹ Mulungu anawonekela futi ku Shilo , pakuti anaziulula kuli Samweli nu Shilo kupitila mu mau.

Chapter 4

¹ Mau a Samweli anabwela kuli Israeli yonse . Apa Israeli anayenda kuja kunkhondo kukamenyana ma Philistini. Anamana misasa Elbeneza , koma ma Philistini anamanga wisasa pa Apheki. ² A Philistini anatanthama mumunzele kumenyana na Israeli anamenyedwa na ma Philistini , wamene wanapaya amuna kuwelengela pa fupi kukwana folo sauzande pamalo pamene wanamenyalama. ³ Pamene wanthu wanabelela pamusasa, wakulu wa Israeli wanati , "Nchifukwa chani Yehova atigonjesa lelo pamenso pama Philistini ? " Lekenitilete chombo chachipangano cha Yehova kuno kuchokela ku Shilo , pakuti chizankhala kuno na ife , kuti chingatunge m'chitezezo kuti chosa mumanja yawadari wathu." ⁴ Apo wanthu ana tumako wamuna ku Shilo kuchokela uko wananyamula bokosi yachipangano ya ambuye Yehova wamene amankhala pamwamba pa ma cherubimu. Anyamata wabili wa Eli , Hophini na Phineyas , wanali kwamene na bokosi yachipangano ya Mulungu. ⁵ Pamene bokosi yachipangano cha Yehova inafika pamusasa , wonse wanthu waku Israeli anakuwa maningi , nanthaka inavomekeza kukuwa kwao. ⁶ Pamene ma Philistini anamvela chongo kamba kakukuwa , wanakamba kuti , " Uku kukuwa mokweza mumisasa ya a Heberi kutanthauzani ? " Pamene apo anaziwa kuti bokosi yachipangano ya Yehova inali ya fika mu misasa. ⁷ A philistini anachita mautha; nakukamba kuti , " Mwangena kamulungu mumusasa . " Wanakamba kuti , " Soka kwa ise ! kukalibe kuchitikapo va so kumbuyo konse uku ! " Soka kwa ise ! Ndani azatichingilila kuli iyi milunguyamphamvu? Aya nimilungu yamene yanayamba kumenya aku Egypito na vilango vambili vosiyanasiyana musanga . ⁹ Limbikani, ndipo munkhale wamuna weniweni , ndipo mumenyane." ¹⁰ Ma Philistini wanamenya ,nkhondo , ndipo Israeli anagonjesewa. Munthu aliyose anathawila kunyumba kwake , ndipo wopayiwa wanali wambili maningi ; ndaba sate sauzande masoja woyenda pansi wakugulu ya Israeli wanafa. ¹¹ Bokosi yachipangano ya Yehova inapokewa , na bana bawili wamuna wa Eli , Hofini na Phiniyasi wanafa. ¹² Mwamuna wakutundu wa Benjamini anathawa kuchokela pamuzele wankhondo nakubwela ku Shilo yamene iyi siku , anafika navovala vake vong'ambika na lukungu mumutu mwake. ¹³ Pamene anafika , Eli anali nkhalapa mpando wake mbali mwa musewu kuyanganila chifukwa mutima wake unanjenjemela nankhawa pa bokosi yachipangano cha Mulungu. Pamene uyu mwamuna ana lowa mu tawuni naku peleka uthenga , tawuni yonse inalila mokuwa. ¹⁴ Pamene Eli anamvela chongo cha kulila kwamphamvu anati , " Tanthauzo yake ya uku kupunda kwa pamwamba maningi nichani?" Munthu uja anabwela mofulumila nakumuwuza Eli. ¹⁵ Apo Eli anali na Zaka nayinte - eyiti musinkhu wake ; Menso yake siyanali kuyang'ana moukhazikika ndipo sienzekuwona. ¹⁶ Munthu uja anati kwa Eli , "Ndine mwamuna wamene wabwela kuchokela kumuzele wankhondo . Nathawa kuchoka kunkhondo lelo. "Eli anati , zayenda bwanji, mwana wanga?" ¹⁷ Mwamuna analeta nkhan yachilendo anayankha na kunena kuti , " Israeli anathawa ma Philistini , Ndipo pankhala kumenyewa kukulu maningi pawanthu wathu. Nafuti , wana banu babili wamuna Hofini na Phineyasi , wafa , ndipo chombo chachipangano cha Mulungu chapokewa." ¹⁸ Pamene anatomola chombo cha Mulungu Eli anagwa chagada kuchoka pampando wake pambali pa geti . Mkosi wake unatyoka , ndipo anafa , chifukwa anali wokalama na kulema . Anaweluzwa Israeli kwa zaka fote. ¹⁹ Ano mpongozi wake , mkazi wa Phineyasi , anali na mimba na kusala pang'ono kubala . Pamene anamvela nkhan yachilendo kuti bokosi yachipangano ya Mulungu inagwiriwa nakuti apongozi wake ndiponso wamuna wake wanafa , anagwada nakubala , koma ululu wapo bala unamukulila. ²⁰ Atasala pang'ono kufa azimayi wamene wanali kumuthandiza wanakamba kuti kuli yeve , "Osayopa ndaba wabala mwana mwamuna ." Koma sanayankhe kapena kuikako mutima kuli vamene wanakamba. ²¹ Anamuteya mwana zina yake Ikabodi, kukamba kuti , "Ulemelelo wachokamo mu Israeli " pakuti chombo cha Mulungu chinatengewa mwachikakamizo, ndiponso chifukwa cha bapongozi wake na mwamuna wake. ²² Iye anati , " Ulemelelo wa Mulungu wachokamo mu Israeli , chifukwa bokosi yachipangano ya Mulungu yapokewa mwa chikakamizo."

Chapter 5

¹ Apa ma Philistini wana poka chombo chamulungu mwachikakamizo , naku chichosa ku Ebeneza kuchibwelesa ku Ashdodi. ² Ma Philistini wanatenga chombo cha Mulungu , nakuchileta mu nyumba mwa Dagoni kunkhazika pafupi mumbali mwa Dagoni . ³ Pamene banthu baku Ashdodi wanauka kuseniseni siku yokankhapo , Dagoni anapeza agwa choyang'ana chinso pansi pafupi na chombo cha chipangano cha Mulungu . Apo banatenga Dagoni nakumunkazika bwino mumalo mwake futi. ⁴ Koma pamene wanauka kuseniseni mumawa mokonkhapo , onani, Dagoni anali atagwa , choyang'ana chinso chake pansi , pa fupi na chombo cha Yeheva . Mutu wa Dagoni namanja yake yonse yabili yawali gone yonyonsoka , kufupina chiseko. Chimubili chabe cha Dagoni ndiye chinasalako. ⁵ Ichi nichu fukwa chake , olo lelo , wansembe wa Dagoni na aliyense wamene amabwela munyumba mwa Dagoni samadyakapo pansi pamalo pangenela muli Dagoni ku Ashdodi. ⁶ Kwanja kwa Yehova kunalema maningi pali banthu waku Ashdodi . Anawaononga nakuwalanga navipute , konse kubili , mu Ashdodi na pa wapa fupi na malile wake. ⁷ Pamene banthu aku Ashdodi wanaziwa zamene zenzochitika , anakamba kuti , " Chombo chachipangano cha Mulungu wa Israeli sichifunika kunkhala na ise , ndawa kwanja kwake kwakosapo kusushana naife ndiponso mususana na Dagoni Mulungu wathu." ⁸ Apo wanayitana nakuyika pamusonkhano umozi wonse mwa osogoleli wa ma Philistini ; anati kwa wave, "Tizachita bwanji na chombo cha Mulungu wa Israeli ?" Wanayankha , "Lekani bokosi yachipangano ya Mulungu wa Israeli , ibweleseni ku Gathi. " Apo wananyamula nakupeleka chombo cha Mulungu wa Israeli ku Gathi." ⁹ Koma atabwelesa chija chinthu kuli aya malo , kwanja kwa Yehova kunankhala kumenyana na muzinda uja , kupangisa musokonezo ukulu maningi . Anawakhaulisa wanthu wa kuli uyu muzinda , wonse wang'ono na bakulu; ndipo vipute vinawayamba kumela pamathupi pawo. ¹⁰ Apo wanatumiza ija bokosi ya Mulungu ku Ekironi . Koma kungoti chabe ija aki ya Mulungu ya fika mu Ekironi , wamu Ekironi wanalila mokuwa kuti , "Waleta kwa ise aki ya Mulungu wa Israeli kuti watipaye pamozi na banthu wathu . " ¹¹ Chomcho wanayitana nakusonkhanisa pamozi wonse azisogoleli wa ma Philistini ; anati kwa weve , " Tumizani kutali aki ya Mulungu wa Israeli , ndipo lekani ibwelele kumalo wake - wake , pakuti isatipaye ise na banthu bathu." Ndawa kwenze mpanipani wa imfa mu muzinda wonse ; ndipo kwanja kwa Yehova kunalema maningi kuli aya malo. ¹² Wanthu wamene siwanafe anakhaulisidwa na vovimba , ndipo kulila kwa muzinda uja kunakwera kumwamba kumitambo.

Chapter 6

¹ Apa aki ya Yehova inali muziko ya ma Philistini kwa myezi seveni. ² Manje banthu wa mutundu wama Philistini wanayitanisa ansembe na wowombeza ; anati kwa weve , "Tifunika tichite bwanji na aki ya Mulungu ? Tiuzeni mwamene tizatumizila poyibweza kumbuyo kuziko kwawo." ³ Ansembe na wowombeza anati , " Ngati muzabweza aki ya Mulungu wa Israeli , osayitumiza palibe chopeleka ; munjira iliyonse mutumizileni chopeleka chovomekeza kulakwa . Chokonkhapo muzachilisidwa , ndipo muzaziwa nichu fukwa chanji sanalekeze kuku menyani imwe mpaka namanje." ⁴ Apo wanakamba kuti , " Tipeleke mtundu wabwanji wa chopeleka chovomelela kulakwa kwathu pomubwezela ?" Anayankha kuti , " Mabola fayivi yagolide , tumbewa towumbiwa na golide tuli fayivi , fayivi inkhare namba yamene iyimilila ma fumu yachi Philistini pakuti naweve wali fayivi . Chifukwa matenda yamozi na yamozi yapalana yonakudwalisani imwena asogoleli wanu. ⁵ Chomcho mufunika kupanga vopalanisako ku vovimba vovimba vanu , navopalanisilako tunyama twanu twamene tumaononga aya malo yanu , nakupeleka ulemelelo kwa Mulungu wa Israeli . Kapena azanyamula wakuchosapo kwanja kwa chilango pali imwe ; pa mulungu yanu , na kuchoka mu yano malo yanu. ⁶ Nichifukwa chani imwe mufuna kukosesa mitima yanu , monga a Egipti na Farawo wanalimbisa mitima yawo ? Ndiye pamene Mulungu wa Israeli ana anachita nawo mwankhanza maningi; kodi a Egipti sanawa pitikise wanthu ndipo wana choka? ⁷ Apa manje , konzani chikochikale cha nyowani na ng'ombe ziwili zikazi zonyansha wana zamene zikalibe kumangiwapo kale. Mangani izi ng'ombe pa chikochikale , koma pelekani tuwana twake kunyumba kutali na mai wake. ⁸ Chokonkhapo mutenge aki ya Yehova nakuyika muchikochi. Ikani vowumba vagolide vovomelela mulandu vamene mumubwezela , mu bokosi kumbali imozi pa fupi na aki ya Yehova . Ndipo muyitumize nakuyilekelela iyende kwao. ⁹ Pambuyo pake mulindilile; ngati izayenda kukwezeka mpaka kuziko kwawo ku Bethi shemeshi , nishi ni Yehova wamene anakwanilisa kuchita ichi chionongeko koma ngati iyayi , ndiye pamene tizaziwa kuti sikwanja yake yamene inatipasa chilango kuti chinango tichitikila chabe mwangozi yotipezekeza." ¹⁰ Waja amuna anachita monga mwamene anawauzila . Anatenga ng'ombe ziwili zonyonsha , nakuzimanga pa chikochikale, nakusunga tuwana twake kunyumba. ¹¹ Anayika aki ya Yehova muchikochi , pamozi na bokosi yamene muna mbewa zowumbiwa na golide na vowumba vama bola va golide. ¹² Ng'ombe zinayenda steleti molungama njira yaku Bethi Shemeshi . Zinayenda mokonkha njila imozi yikulu , apo zinali kulila modandaula pamene ziyenda , ndipo sizinali kukonekela munsanga kuyenda kurayiti kapena kumalefuti. Azisogoleli ama Philistini anali kukonkha muwambuyo mpaka ku Bethi Shemeshi. ¹³ Iyi nthawi wanthu waku Bethi Shemeshi wanali kuchosa wheati mu malo yakufupi na manzi . Pamene ananyamula menso yawo nakuwona aki ya Yehova anasangalala. ¹⁴ Chija chikochi chinafika popitila mumunda mwa Yoswa wochokela ku tawuni ya Bethi Shemeshi na kuyimilila pamene paja . Penze chimwala chikulu maningi pamene apo , ndipo waja wanthu wanapandula mapulanga wakuchikochikale , na kupoleka zija ng'ombe monga usembe yo shoka kwa Yehova . ¹⁵ Alevi anaselusa pansu aki ya Yehova na bokosi yamene yenze pamozi nayo, mwamene munali zisauzo zagolide , nakuviyika pachimwala chikulu . Amuna aku Bethi Shemeshi anapeleka chopeleka choshoka namulilo nakupeleka nsemb siku yamene iyo kwa Yehova. ¹⁶ Pamene azisogoleli ali fayivi wana Philistini anawona ichi , wanabwerela yamene iyi siku ku Ekironi. ¹⁷ Ivi nivovimba va golide vamene ma Philisti anabweza kuvipanga chopeleka chovomelela mulandu kwa Yehova chimozi chaku Ashdodi , chimozi cha ku Gaza , chimozi chaku Ashkeloni , chimozi chaku Gathi , na chimozi chaku Ekroni. ¹⁸ Mbewa zangolide zinali zolingana mu namba monga nichiwelengelo cha mizinda yonse ya ma Philisti yenze yama fumu osogolela , pawili ponse, mizinda yo chinjilidwa na minzi yamene yanali musanga . Chimwala chikulu chamene wanankhazikapo aki ya Mulungu , chinankhalilila nimboni mpaka siku yalelo mumunda mwa Yoswa mu Bethishemayiti. ¹⁹ Mulungu anawayamba kuwamenya wanthu wenangu waku Beth Shemeshi chifukwa anayang'ana mu chombo cha Yehova . Anapayapo fite sauzande na sevine amuna . Wanthu analila chifukwa Yehova anawapasa nkonya ikulu maningi . M'malo mwa wanthu 50,070 amuna , zinabwela zalembewa pasogolo pake na mamasulidwe yamakono , yama lembewa kuti sevine amuna. ²⁰ Wanthu waku Beth Shemeshi banati , "Ndani wamene akwanisa kuyimilila pa menso pa Yehova , uyu mulungu woyela ? Aki ya Mulungu izayenda kuli ndani ikachoka kuli ise?" ²¹ Anatuma anthege ku wanthu wankhala ku kinathi Jearimu , " kunena kuti ." A Philisti wabwelesa aki ya Yehova ; selukani mubwele muyinyamule muyibweze kwanu . "

Chapter 7

¹ Wanthu waku Kiriathi Jearimu wanabwela nakutenga aki ya Yehova, nakuyileta munyumba mwa Abinadabu yamene inali pa lupili . Anayika padela mwana wake mwamuna Eleaza kuti azisunga chombo cha Yehova. ² Kuchokela pamene aki ya Yehova ina nkhalu mu Kiriathi Jearimu , pana pita nthawi itali , zaka twenti. Yonse nyumba ya Israeli inalila modandaula na kukambila kubwelela kwa Yehova. ³ Samweli anati kwa anyumba yonse ya Israeli , " Ngati muzabwelela kwa Mulungu na mutima wonse , chosani milungu yachilendo na ma Ashtorethi yamene yali pakati panu , tembenukilani mitima yanu kuli Yehova , nakupembeza yeve yeke , ndipo azakuleselelani kumanja manja yama Philisti." ⁴ Apo wanthu wanu Israeli wanachosa ma Bala nama Ashtorethi , nakupembeza Yehova yeka . ⁵ Samweli anati , "Waleteni pamozi wonse a Israeli ku Mizipa , ndipo ine nizakupemphelelani kuli Yehova ." ⁶ Wanakolongana pa Mizipa , nakutaya manzi nakuyatila pa menso pa Yehova . Wanasala zakudya ija siku nakukamba kuti , "Tachimwila Mulungu. Nikwamene uku kwamene Samweli anaweluza mikangano ya banthu ba Israeli nakuwasogolela. ⁷ Sopowo ma Philistina yanamvela kuti wanthu waku Israeli wanasonkhana ku Mizipa , asogoleli wa ma Philisti anayamba chipongwe kumenya Israeli . Pamene wanthu waku Israeli wanamvela ichi , anayopa ma Philistina . ⁸ Chokunkhapo wanthu waku Israeli wa nati : Kwa Samweli , " Osaleka kuyitana mokuwa kuli Yehova Mulungu wanthu kuti pemphelelako pakuti atipulumuseko ku manja yama Philisti." ⁹ Samweli anatenga kambelele kamene kanyonsha mwana nakukapeleka konse kankhala chopeleka choshoka kwa Yehova , pambuyo pake Samweli anali mokuwa kwa Yehova kulilako banthu wa mu Israeli . Ndipo Mulungu anamumvela nakumuyankha. ¹⁰ Pamene Samweli analikupeleka chopeleka choshoka pamulilo , a Philisti wana fendela nakuyamba ndewo wanthu waku Israeli . Koma Yehova anagunda ngati kaleza mokuwa maningi ija siku mosusana na ma Philistina nakuwa ponya mumu sokonezo , ndipo wananyuka mumenso mwa Israeli. ¹¹ Amuna aku Israeli wanachokela ku Mizipa nakuwapitikisa ma Philisti nakuwapaya mpaka kuyenda kufika kunyansi kwo Bethi Kara. ¹² Kuchoka apo Samweli anatenga mwala nakuwayika pakati pa Mizipa na Schemi . Anayitana zina yake kuti Ebeneza kukamba kuti , "Kufika apa Yehova atithandiza." ¹³ Apo ma Philisti wana chimfishiwa ndipo sanalowe muboda ya Israeli . Kwanja kwa Mulungu kwenze kushushana na ma Philisti masiku yonse ya Samweli. ¹⁴ Matawuni yamene yenze yanatengewa mwachikakamizo nama Philistina kupoka Israeli yana bwezewa kuli Israeli , kuchokela ku Ekroni mpaka ku Gathi ; Israeli anapoka nakubwezela malile yamalo yako yonse kupoka ma Philistina. Ndipo panankhala mtendela pakati pa Israeli na ma Amoriti. ¹⁵ Samweli anaweluza waku Israeli yonse masiku ya moyo wake. ¹⁶ Chaka chilichonse anali kupitamo mozunguluka kuchokela ku Bethelo . Ku Giligai , na Mizipa . Anali kuweluzwa milandu ya Israeli mumalo yonse aya. ¹⁷ Ndipo anali kubwelelano ku Rama , chifukwa nyumba yake inali kwamene kuja ; nakweve futi analikuweluzwa mikangano ya pakati pa Israeli . Kwamene uku anamanga guwa ya Yehova.

Chapter 8

¹ Pamene Samweli anakalamba anasankhala bana bake wamuna kunkhala woweluza wamu Israeli. ² Zina ya mwana wake wayamba inali Yoweli , ndipo Zina ya mwana wake wa chibili anali Abija . Wanali woweluza milandu ku Beenshiba . ³ Wana wake siwanali kuyenda munjila za watate wawo , koma wanali kusakila malipilo yaukhuluku . Wanetenga ziphuphu nakukhotesa chilingamo. ⁴ Chokonkhapo wakulu wakulu wonse waku Israeli wanakolonganikana pamozi nakubwela kuli Samweli ku Roma . ⁵ Wanakamba kuli yeve , kuti, "Yang'ana , iwe wakalamba , koma bana nako sibayenda munjila zako . Tisankhile mfumu yamene izatiweluzwa monga mayiko yenangu yonse. ⁶ Koma sichinamukandwelese Samweli pamene wanakamba kuti , " Tipase mfumu yamene izitiweluzwa . " Ndipo Samweli anapemphela kwa Yehova . ⁷ Yehova anati kwa Samweli , " Umveleliwu ya banthu muli vonse vamene wakamba kwa iwe ; ndawa siwanakukane iwe , koma wakana ine kuti nisankhala mfumu yawo kuwalamulila. ⁸ Manje wachita chimozi mozi mwamene wanachitila kuchokela siku yamene ninawa chosa mu Egiptito, kunisiya ine , naku tumikila milungu , ndipo nimwamene wachitila nakuli iwe futi. ⁹ Apa manje wamvelelele, koma uwachenjeze maningi ndipo leka waziwe injila yamene mfumu izakawalamulilamo." ¹⁰ Mwa ichi Samweli anawauza yonse mau ya Yehova ku wanthu wamene wanali kupempha ku pasiwa mfumu. ¹¹ Anati , "Uyu ndiye uzankhala mwambo wa mfumu iliyonse yamene izayamba kuku lamalilani azatenga wana wana wamuna nakuwapasa mandindo kumagalimoto yankhondo ndipo anzankhala muna oyendeswa wa hosi nakuthamanga pambuyo pamagaleta ake. ¹² Azazi sankhala yeka makapitawo wa ma sauzande na ma kapitawo wa ma fifite . Azaka yika winangu wolima munda wake , wenangu wochosa va mumunda , ndipo wenangu wopanga zida zake zankhondo nawenangu wopanga visulo vakumagaleta yake . ¹³ Azakatenga wana wanu akazi kunkhala wa mape fyumu , makhukhi , na wa mu bekali. ¹⁴ Azakatenga minda yanu yabwino maningi , madimba yampesa na ma ochadi ya oliva , na kuvipasa kuli anchito wake. ¹⁵ Azatengapo gawo yachikhumi pa zamumunda zanu zopangila afa na zipaso zamumadimba mwanu nakuzipasa kuma offisala na kuli wanchito wake . ¹⁶ Azatenga wanchito wanu wamuna na wakazi na zabwino maningi pa ng'ombe zanu{ Malembedwe yachi Heberi ingawelengewe kuti amuna achinyamata m'malo mwa ng'ombe } na madonkhe yanu azavipanga vonse kumusewenzela. ¹⁷ Azakatenga gawo yachikhumi pa pavinyama vanu ndipo muzankhala akapolo wake. ¹⁸ Apo pasiku iyamusango uyu muzalila mokuwa chifukwa chamfumu yanu yamene mwazisankhila mweka ; koma Yehova sazakuyankhani pasiku ija . " ¹⁹ Koma wanthu anakana kumumvelelele Samweli anati , " Iyayi ! pafunika kunkhala mfumu yotilamulila ise. ²⁰ Pakuti tingankhale monga mayiko yenangu yonse , na pakati fumu yatu inga zitiweluzwa ise nakuyenda pa sogolo kutimenyela nkondo zathu." ²¹ Pamene Samweli anamvela mau yonse yawanthu anayabwezapo mumatu mwa Yehova. ²² Yehova anati kwa Samweli , " Wamvelele mau yawo ndipo pangis kuti winangu ankhale mfumu yawo ." Apo Samweli anati kuli wanthu waku Israeli , "Munthu aliyonse afunika ayende kumuzinda wakwawo."

Chapter 9

¹ Kunali munthu ochokela ku Benjamini, mwamuna wochuka. Zina yake anali Kishi mwana wa Abiele mwana wa Zelolo mwana wa Beconathi mwana wa Aphiya , uja mwana wa mu Benjamayiti. ² Anali na mwana mwamuna zina yake Sauli , m'nyamata wokongola . Kunalibe munthu pakati pawanthu waku Israeli wamene anali wakongola manngi kupambana uyu munyamata . Kuchokela mumapewa ake kuyenda kumutu anali mutali maningi kupambana munthu wina aliyonse . ³ Apo madonke ya Kishi , tate wake wa Sauli , yanali yatasowa . Apo Kishi anati kwa Sauli m'nyamata wake , "Tengapo m'mozi mwa wanchito uyendenaye , nyamuka ndipo yenda kusakila madonke." ⁴ Manje Sauli anapitila njila yamumalipili ya Ephremu nakuyenda kupitila mumalo yaku Shalisha , koma sanayapeze . Pasogolo pake anapitila mumalo ya ku Shaalimu , koma malaweve kunalibe yaja madonke. Chokonkhapo wanapitila mumalo yakuma Benjamayiti , koma nakweve kunalibe sanayapeze. ⁵ Pamene wanabwela kumalo yaku Zufu , Sauli anakamba kuli wanchito wake wamene analinaye kuti , " Tiye tibwelele , ngati sitizachita ichi wa tate wanga wazaleka kudandaula ma donke nakuyamba kutasikila." ⁶ Koma wanchito anawena kuti kwa yeve , " Nimvele , muli munthu wa Mulungu muli uyu muzinda . Nimunthu wamene amapasiwa ulemu ukulu maningi ; chilichose chamene akamba chimachitika zooni . Tiye tiyende ; kapena azatiuza tipitile njila yiti paulendo wathu . " ⁷ Apo Sauli anafunsa wanchito wake , "Manje ngati tizayenda timupelekela chani munthu wa Mulungu ? Kawili buledi yenze mumathumba yathu yamasaka yasila , ndipo palibe mphaso yapasa munthu wa Mulungu . Tili na chani?" ⁸ Wanchito anayankha Sauli kuti , pano nili na mpimo umozi mwa vigawo folo va ma shekelo ya siliva yamene nizapasa munthu wa Mulungu , kuti atiuze njila yamene tizayendela paulendo wathu. ⁹ (Palamulo mu Israeli , pamene munthu anayenda kufunsa nzelu za Mulungu , anali kunena kuti bwerani tiyeni kuli wa menso mphenya . " Pakuti aneneli amasikuwano kudala anali kuwayita kuli wamensomphenya.) ¹⁰ Apo Sauli anati kuwanchito wake , " Wakamba bwino . Bwela , tiye tiyende . " Basi wanayenda mumuzinda mwamene munthu wa Mulungu anali kunkhalamo. ¹¹ Pamene anali kuyenda mokwezeka impili mumuzinda , anapeza asikana wachokela mumuzinda kubwela kutapa manzi , Sauli nawanchito wake anati kufunsa , "Aliko woyang'ana kuno?" ¹² Banayankha nakunena kuti , " Aliko ; onani , alipasogolo panu . Fulumilani, ndawa abwela lelo mumuzinda , ndaba wanthu lelo waza peleka nsembe pa malo apamwamba. ¹³ Mukango lowa mumuzinda muzamupeza , akalibe kuyenda kukwela kumalo ya pamwamba kuyenda kudya. Banthu siwazadya mpaka afike , chifukwa azadalisa nsembe ; kuchoka apo waja woyitaniwa wazadya . Apa yendani , pakuti muzamupeza musanga - musanga." ¹⁴ Choncho wanayenda mumuzinda , pamene wanali kulowa mumuzinda weve wana Samweli abwela kwamene wenze lili mowa lungama , Kuti ayende ku malo apamwamba. ¹⁵ Manje siku imozi Sauli akalibe kufika , Yehova anali ataulula kuli Samweli: ¹⁶ "Mayilo monga thawi zino ine nizatuma mwana wachichepele kuchokela kuziko ya Benjamini ndipo uzamuzoza kuti ankhale kazembe wolamulila wanthu wanga Israeli . Aza pulumusa wanthu wanga kuwachosa mumanja ya ma Philistina chifukwa nawayang'ana wanthu wanga na chifundo chifukwa kuyitana kwao kufuna thandizo kwa fika kuli ine." ¹⁷ Pamene Samweli anaona Sauli , Yehova anamuuzwa , "Alipano munthu wamene ine ninakuuzapo ! " Niyeye wamene azalamulila wanthu wanga." ¹⁸ Pasogolo pake Sauli anabwela pa fupi na Samweli mu geti nakukamba kuti , "Niwuzeni koni ilikuti nyumba ya m'neneri?" ¹⁹ Samweli anayankha Sauli kuti , " Ndine wamenso mphenya . Kwelani pasogolo panga kumalo apamwamba , pakuti lelo iwe nzadye na ine. M'mawa nizakulola kuti uyende , ndipo nizakuwuzwa zonse zamene zili mu mutima wako . ²⁰ Kukamba zamadonke yako yamene yanasowa masiku yatatu yapita , osadankhawa za weve ,pakuti yapezeka . Ndipo nipali ndani pali zakumbwa zonse za Israeli? Sipali iwe na wonse wakunyumba ya tate wako?" ²¹ Sauli anayankha kuti , "Sindine waku mutundu wama Benjamiti , kuchokela kuli mutundu wung'ono maningi wamu Israeli ? kodi mukoka wanga sindine ung'ono maningi pa mikoka ya pa mutundu wama Benjamini ? Lomba nichu fukwa chanji kuti mwakamba kuli ine munjila yamusango uyu?" ²² Apo Samweli anatenga Sauli nawa nchito wake nakuwaleta muchipinda chikulu nakuwa nkazika pamalo yapamatu ya waja wamene wanayitaniwa wonse pamozi wanali pafupi fupi wanthu thirti. ²³ Samweli anati kwa khukhi , "Letani chigawo chamene ninakupasani , chamene ninanepo kuli imwe kuti ikani pambali . " ²⁴ Apo khukhi analeta chibelo na zonse nyama zamene zenzepo na kuyika pamene panali Sauli . Chonkonkhapo Samweli anati , " Ona zenze zosungiwa zaikiwa pali iwe. Idya , chifukwa yenze yasungiwi iwe mpaka nthawi yoyikika ikwane , kuchokela pa nthawi yamene yamene ninakamba kuti , ' Nawayitana wanthu . " Apo Sauli anadya na Samweli siku ija. ²⁵ Pamene wanaseluka kuchokela kumalo yapamwamba mumuzinda , Samweli ana kamba na Sauli pamutenge wa nyumba pamwamba. ²⁶ Ndipo pakutulukila kwa mbandaku cha , Samweli anayitana Sauli pamwamba pa mutenge wanyumba na kunena kuti , " Nyamuka kuti nkutume kwanu ndipo Sauli anauka , ndipowonse awili iye na Samweli anayenda kunja mumusewa. ²⁷ Pamene anali kutulukila kunja kwa muzinda , Samweli anati kuli Sauli , "Muwuzwa wanchito wako kuti asogoleko ulwendo pasogolo pa ife -

" ndipo ana fende pasogolo-" Koma iwe uyenela kusalila kuno pakanthawi , pakuti ninga ulule uthenga wa Yehova kuli iwe."

Chapter 10

¹ Manje Samweli anatenga chikho cha mafuta , nakuthira pamutu pa Sauli , nakumu muyontha kissi. Anati, "Kodi Yehova sanakuzoze iwe kuti unkhale musogoleli wa wolamulila chokolo chake?" ² Mkasiyana na ine lelo , uzapeza amuna abili pa fupina manda ya Recho , mumalo ya Benjamini pa Zeliza . Weve wazakamba kuti kwa iwe , ' madonke yamene wenzo sakila yapezeka . Apa manje batate bako waleka kusakila madonke koma ada nkhwaza iwe , akuti, "Nizachita bwanji pali mwana wanga?" ³ Koma uza pitililako kuyenda kuchokela apo, ndipo uzafika kumutenga wa oaki waku Tabori . wanthu watatu oyenda kwa Mulungu pa Bethela azaku mana naiwe pamene paja , m'mozi wonyamula tumbazi tung'ono tutatu winangu wonyamuna mikate itatu. Na winangu wonyamuna thumba yachakukumwa. ⁴ Wazakuposha nakukuposa mikate ibili yabuledi , yamene uzalandila kuchoka mumanja mwawo. ⁵ Zitapita izo uzabwela ku phili ya Mulungu , pamene kagulu ka asilikali wazida wa m'tundu wama Philisti kalili. Pamene uzafika pali uyu muzinda ,uzakumana nagulu ya aneneri ilikuseluka pansi kuchokela kumalo yapamwamba ali na choyimbila choumbidwa moponyongola , tambolini , mutolilo , na uta wa tunthambo woliza ; azapezeka navo azankhala ali kunenera . ⁶ Muzimu wa Mulungu azakuntha maguduka pali iwe , ndipo uzanenera nawo , nakuti uzachingiwa kusanduka munthu winangu . ⁷ Apo pemene izi zizindikilo zizabwela pali iwe , uchite chilichonse chamene manja yako yazakwanisa kuchita , pakuti Mulungu ali naiwe. ⁸ Seluka mumanso mwanga kuyenda ku Giligali . Pambuyo pake ine nizabwera kuselukila kwa iwe kupereka vopeleka voshoka nakupeleka nsembe ya chopeleka chamutendele . Ukayembekezele pa masiku yali seveni mpaka nikabwele kwa iwe kukuonesha vamene ufunika kuchita . " ⁹ Pamene Sauli anapiliwuka kuchoka pali Samweli , Mulungu anamupasa mutima winangu . Ndipo izi zizindikilo zonse zina kwanilisika yamene ija siku. ¹⁰ Pamene wana fika pa tupolo , gulu ya ananeli inaku mana naye , ndipo muzimu wa Mulungu unamu gudukila kwakuti ananewera pamozi nawa. ¹¹ Pamene aliyense anamuziwa kudala anamuona anewera pamozi na aneweri banthu wanakambisana kuti , "Nichani chamene chachitika kuli mwana wa Kishi ? Kodi Sauli naye nimumozi wa aneneri manje?" ¹² Munthu wamene anachokela naye kumala amozi anayankha kuti , "Ninshi tate wawo ndani?" Chifukwa cha ichi , ayamau yanasanduku mwambi wakuti, " Kodi Sauli naye nimumozi wa aneneri?" ¹³ Pamene anasiliza kusesema anabwera kumalo apamwamba . ¹⁴ Apo malume wake Sauli anati kuli yeve wawanchito wake , " Mwenze mwayenda kuti?" Iye anayankha , "Mukusakila madonke ,pamene tinaona kuti sitinaya peze , tinayenda kuli Samweli." ¹⁵ Malume wake Sauli anati , "Chonde niwuzenikoni chamene Samweli anakamba kuli imwe ." ¹⁶ Sauli , anayankha kuli bamalume bake , "Anatiuza potuwa kuti madonke yanali yatapezeka ." Koma anabisa zaukhani yo khuza zaumfumu, yamene Samweli anakambapo. ¹⁷ Samweli anayitana wanthu pamozi pamene pa Mulungu pa Mizipa. ¹⁸ Anati kuli a Israeli , "Ichi ndiye chamene akamba Yehova , Mulungu wa Israeli : 'Ninatulusa Israeli kunja kwa Egypti , nakukupulumusa iwe kuchoka mukwanja kwa ma Egypto , namukwanja kwa maufumu onse yamene yanali kukupondeleza iwe.' " ¹⁹ Koma lelo mwakana Mulungu wanu , wamene anakuleselelani imwe kuli yonse mavuto na zo sausa ; ndipo mumakamba kuti kuli eve , " Tinkhazikileni mfumu yoti lamulila ise . ' Manje zileteni mweka pamenso pa Yehova kukonkha mitunda na viwongo." ²⁰ Choncho Samweli analeta yonse mitundu ya Israeli pa fupi , ndipo mutundu wa Benjamini unasankhiwa . ²¹ Ndipo analeta mutundu wa Benjamini pa fupi kukonkha viwongo . Ndipo mukoka wa Matriti unasankhiwa ; naye Sauli mwana wa Kishi anasankhiwa . Koma pamene wana yenda kuwusakila sanapezeke. ²² Apo wanthu anali kufuna kufunsa Mulungu mafunso yambili , " Kodi kukali munthu winangu wamene a funika kubwela ?" Mulungu anayankha , "Wazibisa yeka pavi katundu va machola." ²³ Apo wanathawa nakuyenda kumu fukulula Sauli kuchoka pamene anliti . Pamene anaimilila pakati pa wanthu anali mutali kuchilapo wonse kuchokela mumapewa kuyenda kumwamba . ²⁴ Ndipo Samweli anati kuli banthu , "Mumuona munthu wamene Yehova asankha ? Palibe winangu futi pakati pawanthu wonse ! " Wonse wanthu wanakuwa , " Lukhale moyo utali mfumu! " ²⁵ Apo Samweli anauza wanthu myambo na malamulo ya zaufumu , nakuya lemba mubuku , nakuyiyika pamenso pa Yehova pambuyo pake Samweli anatumiza banthu bonse kutali , aliyense kunyumba kwake. ²⁶ Sauli naye anayenda kunyumba kwake ku Gibeya , ndipo anayenda naye pamozi amuna olimba , wamene Mulungu anakumya mitima yawo. ²⁷ Koma wanthu wachabechabe wanakamba kuti , " Nanga uyu munthu azatipulumusa mutundu bwanji ? " Awa wanthu wana pepusa Sauli ndipo sanali kuleta mphaso iliyonse kuli Sauli . Koma sauli anankhala chabe zii.

Chapter 11

¹ Apo Nahashi Amonitianayenda naku chingiliza mwankhondo ku Jabeshi Gilead Amuna wonse waku Jabeshi anati kwa Nahashi , "Pangani chipangano na ise , ndipo tizakutumikila." ² Nahashi mu Amoriti anayankha , "Pali lamulo ya uyu munthu ndiye pamene nizapangila chipangano naimwe , kuti nikukolowoleni monse menso yamu yaku nayiti , pakuti mwanjira iyi nibwelese nsoni kuli ma Israeli wonse." ³ Akulu akulu aku Jabeshi anamuyankha kuti , " Utisiye seka kwo masiku yali seveni poyamba ,pakuti titumize anthenga kuli aya malo yonse ya malile ya Israeli. Apo , ngati kulibe aliyense wamene angati pulumusa ise tiza salenda kuli iwe." ⁴ Anthenga waja wanabwela ku Gibeya , kwamene kunali kunkhala Sauli , nakuwuza wanthu zamene zenze zinachitika . Wathu wonse wanalila mokuwa kwenikweni . ⁵ Iyi nthawi Sauli analikukonkha nkhati kuchoka kunja munda . Sauli anati,"Nichani kulo banthu pakuti walile monga malilo ? " Banamuwuza Sauli chamene wanthu waku Jabeshi wananena. ⁶ Pamene Sauli anamwela chamene wanakamba , muzimu wa Mulungu unamukuntha namphamvu , ndipo anakwiya maningi. ⁷ Anatenga nkhati ziwili , nakujuwajuwa mutudunswa , nakutu tumiza ponse ponse mudela yonse ya Israeli kupitila muli aja athenga . Anati , "Aliyense wamene sazachoka panja kukonkha Sauli na Samweli, ichi ndiye chamene chizachitika kuli nkhati zake ." Apo mantha yoyopa Yehova yanagwera pa wanthu wonse . Ndipo wana chokela panja pamozi monga nimuthu umozi. ⁸ Pamene anawa onkhesa pa Bezeki , wanthu waku Israeli anali atatu aku yuda anli sate sauzande. ⁹ Anati kuli athenga wamene wanabwela , " Muzauza amuna waku Jabeshi Gileadi , kuti mayilo panthawi yamene zuwa izakankhala yokaba maningi , muzaleselelewa ." Apo athenga banayenga nakuwuza banthu waku Jabeshi , ndipo wanakondwela . ¹⁰ Apo banthu waku Jabeshi wanauza Nahashi kuti , mayilo tizasalenda kuli iwe , ndipo ndipo ungatichite ise chilichonse chamene chizakakuonekela bwino kwa iwe. ¹¹ Siku yokonkhapo Sauli anayika banthu muwagulu atatu . Anabwela pakati pa musasa panthawi ya ulondawa m'mawa nakuyamba kumenya ma Amoniti nakuwachilmfya mpaka mpaka pamene kunapya muziwa. Waja wamene wanapuluma wanawazikana , kwakuti kunalibe wanthu kupezeka wasalapo wabili pamozi. ¹² Ndipo banthu banati kuli Samweli , "Enze nindani wamene anakamba , ' Kodi Sauli azitilamulila ise? ' Waleteni banthu , pakuti tiwapaye." ¹³ Koma Sauli anati , "Osapaya munthu aliyense iyi siku , chifukwa lelo Yehova aleselela a Israeli." ¹⁴ Apa Samweli anati kuli Banthu , "Bwelani, tiyeni tiyende ku Giligali tikabwezepo kupanga ziko yolamuliwa na mfumu zobadu kuchokela mubanja yimozi ." ¹⁵ Apo banthu bonse wanayenda ku Giligali naku panga Sauli mfumu pa menso pa Yehova mu Giligali kwamene kuja bana peleka nsembe za mutendele m'menso mwa Yehova , ndipo Sauli na banthu bonse wamuna wa mu Israeli wana sangalala maningi.

Chapter 12

¹ Samweli anati kuli ba Israeli bonse , " Namvelelela kuli vonse vamene mwakamba kuli ine , ndipo wanankhazikisa mfumu pali imwe yokulamulilani. ² Manje , si iyi mfumu ilipano iyenda m'menso mwanu , koma ine nine okalamba na imvi , ndipo , bana wanga bamuna alina imwe . Ninali kuyenda mumenso mwanu kuchokela pa ufana mpaka nalelo. ³ Nili pano , pelekani umboni worususa pamenso pa Yehova na pamenso pa wazozedwa wake . Ninabako nkhwari ya ndani? Ninabako douke wandani ? Nindani wamene ninakhuluka? Ninapondelezapo ndani? Nikuchokela mumanja mwa ndani mwamene ninalandilako chiphuphu kunipofulilako menso yanga ? Pelekani umboni wonisusa ndipo nizachibwezela chamene icho chinthu kwa imwe." ⁴ Weve wanayankha kuti , " Siunatinamizapo ise , siunatipondelezapo ise , kapena kuba chinthu chilichose kuchokela mumanja mwa munthu aliyonse." ⁵ Anati kuli weve , "Yehova nimboni yo susana naimwe , ndipo wozozedwa wake nimboni lelo , kuti palibe chamene mwa eza mumanja mwanga . " Mulungu nimboni. ⁶ Samweli anati kuli banthu , " Ni Yehova wamene anasontha Mose na Aroni , naku bwelesa azi tate wanu kuba imya kuchokela kuziko ya Egypiti. ⁷ Apa manje , zileteni mweka , pakuti ine ningakupatilenikoni pamozi naimwe pamenso pa Yehova , pali zonse zochita zabwino za Mulungu , zamene anachita kuli imwe na a zitate wanu. ⁸ Pamene Yehova anbwela ku Egypiti , ndipo makolo yanu yanalila kwa Yehova , chokonkhapo Yehova anatuma Moze na Aroni , wamene wanasogolela makolo yanu kuwa leta kunja kwa Egypiti ndipo wanankhazikika muli aya malo . ⁹ Koma wanaiwala Yehova Mulungu wao; anawagulisa muma Sisera , kapitawo wa ankhondo aku Hazori , mu manja mwa Philisti , na mumanja mwa mfumu yaku Moabu ; awa wonse anamenyana na makolo wanu. ¹⁰ Analila kwa Yehova na kunena kuti , ' Tachimawa , ndawa taiwala Yehova na kuti tatumikila a Bela ndi a Ashtorethi . Koma apa tileseleleni ise kuchoka mu kwanja kwa adani wathu , ndipo ife tizakutumikilani. ¹¹ Apo Yehova anatuma Jarabu Baala, Bedani , Jephthala , na Samweli , na kukupasani kugonjesa pa adani wanu wonse wokuzungulukani , kwakuti munali kunkhala muchitetezo . ¹² Pamene munaona kuti Nahashi mfumu ya wanthu waku Ammoni anabwela kumenyana na imwe , imwe munatikwa ine . ' Awe ! m'malo mwaka mfumu ifunika kuti lamulila ife ' - angankhale kuti Yehova Mulungu wanu , anali mfumu yanu. ¹³ Manje si iyi mfumu yamene wasankha , yamene mwapempha , ndipo yamene Mulungu akusonthelani manje kuti ikulamulileni. ¹⁴ Ngati muyopa Yehova , kumutumikila , na kumvela mau yake , ndipo musaukile mususa kumulo ya Yehova , ndiye kuti babili monse imwe na fumu yamene ikulamulilani pasogolo panu muza satila Yehova Mulungu wanu. ¹⁵ Ngati simuzamvela liwu ya Yehova koma mu ukile malamulo ya Yehova , nishi kwanja kwa Yehova kuzakankala kosusana na imwe , monga mwamene chinalili kumakola banu. ¹⁶ Loko manje zileteni mweka ndipo muzaona ici chinthu chikulu chamene Yehova azachita mumenso mwanu . ¹⁷ Si siku yobweza tirigu lelo ? Ine nizayitana Yehova , kuti atume mkokomo na mvula . Ndipo imwe muzaziwa na kuwona kuti kuipa ni kukulumaningi , kwamene muna chita pamenso pa Yehova , pazipemphera mweka fumu." ¹⁸ Apo Samweli anayitana kwa Yehova ; ndipo muli yamene iyi siku Yehova anatuma mphenzi na mvula . Apo wonse banthu wanayipa Yehova na Samweli maningi. ¹⁹ Ndipo wanthu wonse anati kwa Samweli , "Pemphelela wakapolo wako kwa Yehova Mulungu wako , pakuti tisafe . Pakuti ise taonjezelapo ichi chimo pamachimo yathu yonse yambili , pozipemphera ise tewene bake mfumu." ²⁰ Samweli anayankha , "Osayopa. Munacita ivi vonse voyipa , koma osacoka kuli Mulungu , koma mutumikile Yehova na mtima wanu wonse. ²¹ Osatembenuka kukonka vinthu vilibe kanthu , vamene vilibe phindu kapena vamene sivingakuleseleleni ndaba vilibe nchito . ²² Chifukwa cha zina yake yayikulu koposa , Yehova sazawakana banthu wake chifukwa chamukondwelesa Yehova Kutu akupangeni imwe kunkhala banthu wake. ²³ Koma kuli ine , sichingachtike kuti nichimwile Mulungu poleka kukupemphelani , m'malo mwake ine nizakuphunzisani njila yabwino ndipo niyolungama . ²⁴ Chabe yopani Mulungu nakunutumikila iye muchonandi na mutima wanu wonse . Ganizilaniponi pa vinthu vikulu vamene anakuchitilani. ²⁵ Koma mukalimbikila kuchita voyipa , babili monse imwe na mfumu yanu muzawanongedwa.

Chapter 13

¹ Sauli anali na zaka thirti musinkhu pamene anayamba kulamulila : Atalamulila kwa zaka fote mu Israeli , ² anasankha amuna thri sauzande amu Israeli . Thu sauzande anali na yeve mu Michmash na mu ziko ya malupili ya Bethle , apo pamene ni ushi chibelengelo cha sauzande imozi chinali na Jonathani mu Gibeya yaku Benjamini . Wonse wosalapo masoja anawatumiza kumanyumba , munthu aliyonse kunyumba kwake . ³ Jonathani anagonjesa ija garrisoni yama Philistini yamene inali pa Gibeya ndipo a Philisti anamvela za ichi . Pambuyo pake Sauli analiza lupenga kupita muziko yonse , nati "Lekani a Heberi amvele." ⁴ Israeli yonse inamvela kuti Sauli anagonjesa garrisoni ya ma Philisti , ndiponso kuti Israeli inasanduka chifungo chowola kuli ma Philisti . Apo masoja wanayitaniwa pamozi kukakumana na Sauli pa Giligali . ⁵ A Philisti anakolongana pamozi kuti na Israeli , nama ngolo yankhondo yali thri sauzande amuna okwana sikisi sauzande amuna woyendesa ngolo , ndipo magulu ankhondo oyenda pansi okwane monga kupaka kwa michenga mumbali mwa nyanja . Anakwela na ku yika misasa pa Michmash , kumawa kwa Bethi Aveni . ⁶ Pamene banthu baku Israeli anaona kuti ali mumavuto - pakuti banthu banali munkawa ikulu kwakuti wanabisana mu vilindi vamumyala , pansi pavichamba , pakati pa myala yong'ambika , mu visime , na mumigodi . ⁷ Benangu bakuli ma Heberi wana tauka kushilya kwa Yolodano ku malo ya Gadi na Gileadi . Koma Sauli enze akati ku Giligali , ndipo banthu bonse wanamu konkha apo wanjema . ⁸ Anayembekeza masiku seveni , nthawi yamene Samweli anayika . Koma Samweli sanabweleko ku Giligali , ndipo banthu wanali kumwazi kana kuchoka kuli Sauli . ⁹ Sauli anati , "Nileteleni chopeleka cho shoka na zopeleka zamtendele ." Ndipo anapeleka nsembe yoshoka . ¹⁰ Pamene ana siliza chabe kupeleka chopeleka choshoka Samweli anafika . Sauli anatulukila panja kuyenda kukamuposha . ¹¹ Apo Samweli anati , "Whachita chani ? Sauli anayankha , "Pamene nenze mona kuti banthu wamali kuchoka kuli ine , nakuti iwe siunabwele mukati mwa nthawi yamene unakonza , ndipo kuti a Philisiti banali watasonkhana pa Michmish , ¹² Ninakamba kuti , " Apa a Philisiti azaseluka kubwela kumenyana na ine pa Giligali , ndipo kuti ine sininapemphe chifundo cha Mulungu , 'apo ninazikakamiza neka kupeleka nsembe ya chopeleka choshoka." ¹³ Apo Samweli anati kwa Sauli , "Wachita zopusa . Siana sunge lamulo ya Yehova Mulungu wako yamene iye anakupasa iwe . Pakuti Yehova pokonkhapo sembe ayendo nkazika ulamulilo wako kwamuyaya . ¹⁴ Koma nomba apa ulamulilo wako siuzapitiliza . Yehova asakila mau thu wamene mutima wake wakonda , ndipo Yehova ana sankhula nakumuyika mfumu yakuti asogolere banthu wake , chifukwa siunamvele chamene anaku lamula ine." ¹⁵ Apo Samweli anayankha kuchokela ku Giligali kuyenda ku Gibeya yaku Benjamini . Apo Sauli anawelenga banthu wamene wanali panali eve wanakwane chiwelengelo capa fupi - fupi sikisi hundredi bamuna . ¹⁶ Sauli , Jonathani , mwana wake mwamuna wa banthu bamene wanalipo pamozi naye , ana salila ku Gebala ya ku Benjamini . Koma ma Philisiti anamanga misasa yawo pa Michmishi . ¹⁷ Woyamba nkhondo wanachokela ku misasa yama Philisiti mumagulu yatatu . Gulu imozi inatembenukila chaku Ophana , ku malo ya Shuala . ¹⁸ Gulu inangu inachayila kona kuyenda chaku sayidi kunali Bethi Haroni , ndipo gulu inangu ina tembenukila kuyenda chakuboda yamene iyang'anana na malo yakumbali kwa manzi ya Zeboyima kuyang'ana cha ku sanga . ¹⁹ Kunalibe wapanga visulo vansombi wamene wanalikupezeka mu Israeli yonse , chifukwa a Philisiti anakamba kuti . "Kapena ma Heberi wangazipangile ma panga na mikondo yawoyawo." ²⁰ Koma onse amuna aku Israeli anajaila kukondo kuyenda kuli ma Philisiti , aliyense kuyenda kunola milomo na ma layeni ya geje , mapiki yawo , katemo kawo namajeko yawo . ²¹ Mutengo unali mipimo yamagulu yabili katatu pasikelo kuti unoleshe mu lomo wa pulawu namapiki , ndipo mnyenso umozi katatu pasikelo kuti unoleshe tukatemo na pakuyondololesha vobowolelako . ²² Apo pasiku ya kumenyana , sikunali kupezeka ma panga na mikondo mumanja mwa m'silikali uli yonse wamene enze na Sauli na Jonathani ; pokhapo Sauli na Jonathani mwana wake ndiye anali kupezeka navo ivi vida . ²³ Garrisoni asilikali ankhondo achi Philisiti inayenda kuchokela panja kukampata kopitilapo kaku Michmashi .

Chapter 14

¹ Siku inangu , Jonatahni mwana wa Sauli anati kuli mung'ono wawonyamula zida zaka zankhonde , "Bwela , ma Philisiti kusayidi kwinangu." Koma sianauze atate bake. ² Sauli andi nkhole mopelela malile ya Gibeya manyansi mwa mutengo wa vizimbili wamene uli mu Migironi . Chiwelengelo chokwana amuna pafupi sikisi handredi anali naye . ³ Pamozi na Abija mwana wa Ahitabu (mbale wake Ikabodi) , mwana wa Pheneyas mwana wa Eli , wansembe wa Yehova waku Shilo , wamene anali kuvala efodi . Wanthu sanaziwe kuti Jonathani anali atachoka kuyenda. ⁴ Kumbali zilikonse zakampata kopitilako kwamene Jonathani enzofuna kuchokelako kuti ayende kufika ku garrisoni yama Philisiti , kunali chimwala chopolika kumbali imozi na kwinangu kumbali futi chimwala chopolika . Imozi songa ya chimwala yinalikuyitaniwa kuti Bozezi ndipo nsongo inangu yachimwala yenze kutaniwa zina yakuti Senehe. ⁵ Nsonga imozi yachimwala chopolika inayimilila kumupoto pasogolo pa Michmish , ndipo inangu inali chakumwela pasogolo pa Gebala. ⁶ Jonathani anati kuli mung'ono mwa osunga ndikinyamula vida vake vankhondo , "Bwela , tiye titaukile ku garrisoni ya awa wanthu wamba wamene walibe mudulidwe . Chingachitike kuti Yehova angatisewenzele mumalo mwathu . Pakuti palibe chamene chingamulese Yehova kupulumusa kupitila muli bambili kapena bang'ono banthu ." ⁷ Wonyamula zida zake zankhondo anayankha kuti , " Chita zonse zamene zili mumutima mwwako . Pitiliza , ona nili na iwe , kukumvela malamulo yako yonse." ⁸ Jonathani anati , "Tizataukila kuyenda kuli aba banthu , nakuziwonesha tewenebake kuli beve. ⁹ Ingati bakakamba kuli ise kuti yembekezani pamene apo mpaka ife tibwele kutaunkila kwe mulili apo tizankhala mumalo mwathu nakusata ukila kwe balili. ¹⁰ Koma angati bazayankha , ' Bwelani kwa ise , ' ndipo pamene tizatanka , chifukwa Mulungu awapasa mumanja mwathu . Ichi ndiye chizankhala chizindikilo kuli ise. ¹¹ Apo bonse babili wanazisokolela kuli garrisoni yama Philisiti . A Philisti anati , "Onani a Heberi wachoka mu vidindi vamene wanazibisamo ." ¹² Apo bamuna wa pa garrisoni banaitana Jonathani na wonyamula zida zake zankhondo , nakunena kuti , bwelani mukwele kuno kwa ise ndipo tizakulangizani chinthu chinangu ." Jonathani anati kuli wonyamula zida wake , "Unikonkhe mumambuyo ine , chifukwa Mulungu wawapeleka mu kwanja kwa Israeli ." ¹³ Jonathani anakwela kumwamba mokalawa pamanja pake na pamendo yake , ndipo wonyamula zida wake anakonkha mumambuyo mwake . Aphilisiti wanapayiya mumenso mwa Jonathani , ndipo wonyamula zida wake anapayako wanangu mumambuyo mwake. ¹⁴ Chipongwe choyamba chamene Jonathani nawonyamula zida wake, bananga , china malo yokwana hafu ekala. ¹⁵ Mwenze kuyopa nakusowa mtendele mumusasa , munsanga , na pakati pa banthu . Nangu gulu yawankhondo na wongenela kwa wene mwa chipongwe inasowa mtendele .Ziko yapansi inanjenjemela , naku soweka mutendela maningi. ¹⁶ Ndipo amalonda wa Sauli mu Gibeya yaku Benjamini anayang'ana , mtambo wa asilikali wama Philisiti unali ku mwazikana ndipo anali kuyenda uku na uko. ¹⁷ Ndipo Sauli anati banthu bamene banzeli naye pamozi , " Belangani ndipo muone wamene palibe pakati pa ise." Pamene wanasiliza kupenda , Jonathani sibanalipo. ¹⁸ Sauli anati kuli Abija , " Letani chombo chachipangano cha Yehova kuno," pakuti panthawi iyi chombo chinali na banthu waku Israeli . ¹⁹ Pamene Sauli akali kukamba na wa nsembe , chongo chamusokoweza na mantha mumusasa wa wa Philisiti chinapitiliza kukulilako . Apo Sauli anati kuli wansembe , "Bweza kumbuyo kwanja kwako." ²⁰ Sauli na banthu bonse bamene wanali naye wanakonkha nakuyenda kunkhondo . Panga iliyonse yama Philisiti inali kusewenzesewa kupayilanako weka weka wakuziko yakwao , ndipo panali musokonezo ukulu maningi. ²¹ Apa waja ma Heberi wamene wanali namaPhilisiti poyambilila , ndipo wanali bayenda nawo mumusasa, olo naweve wana thandizana Israeli wamene wanali na Sauli na Jonathani. ²² Pamene bamuna wonse waku Israeli wamene wenze wanazibisa mumapili pa fupi na Ephurayimu bana mvela kuti ma Philisiti wanali kuthawa , loko naweve wanapilikisako mukumenyana. ²³ Apo Mulungu anapulimusa Israeli muli iyo siku , Nipo kumenyana kunatwalilila kupitilila pa Beth Aveni. ²⁴ Ija siku banthu baku Israeli wanasowa mtendele chifukwa Sauli analapisa banthu njozi nakunena kuti , " Azankhala wotembeledwa munthu wamene azadya chakudya ciliconse mpaka kufika mumazulo panthawi yamene nizankhala nakwanisa ku bwezamo muli badeni banga ." Nchifukwa chake palibe loko umozi wa asilikali wamene andyako molawa chakudya. ²⁵ Manje wanthu bonse wanagena munsanga ndipo munali uchi pansi. ²⁶ Pamene banthu banangena munsanga , uchi unakunkhuluka ,koma panalibe aliyense wamene anayika kwanja kukamwa kwake pakuti banthu banayopa chipangano. ²⁷ Koma Jonathani sienze anamvela kuti atate bako banali bamanga banthu na nyazi . Anagwira kakusonga kandodo yamene inali mumanja mwake nakudya nyamula kwanja kwake nakudya ndipo menso yake yanaseguka . ²⁸ Apo m'mozi mwa wanthu ana kamba kuti , " Atate wake walapilisa banthu mwamphavu nanjazi kukamba kuti , " azakankhala wotembeledwa munthu wamene azadya chakudya pa siku iyi , 'olo kuti banthu wenze wanafookana njala. ²⁹ Apo Jonathani anayankha kuti , "Adadi wanga wapanga vuto muziko. Oma mwamene menso yanga yaseguka nalawako pangono uyu uchi. ³⁰ Chingankhale bwino mtundu bwanji ngati banthu wenze

wadya mwaulele lelo kuchosapo pa vinthu vamene tapoka wadani pomenyana lelo? Ndaba apa manje nchifukwa chake wopayiwa siwanapake maningi pakati pa ma Philisiti. ³¹ Wanayamba kumenyana Philisiti ija siku kuchokela ku Michmashi mpaka ku Aijaloni . Banthu wanalema maningi. ³² Banthu wanathamanga molusa pa vinthu vopoka pankhondo nakutenga nkhusa , ng'ombe natubana twang'ombe , nakuvipayila pansi . Banthu wanavidya pamozi namagazi . ³³ Apo wanamuza Sauli , "Ona , banthu wali kuchimwila Yehova chifukwa cha chakudya pamozi namagazi . Sauli anati, "Mwachita moskhulupilika . Manje kunkhuluzani mwala ukulukuno kuli ine ." ³⁴ Sauli anati , "Yendani kuya pakati pa banthu nakuwauza kuti , " Lekani munthu aliyense alete ng'ombe zake kudya . Osachimwila Mulungu pakudya nyama ili na magazi . Apo munthu aliyonse anabwela na nkhwani yake uja usiku nakuyipaya pamene apo. ³⁵ Sauli anamanga guwa kwa Mulungu yamene inali guwa yake yoyamba yamene anamanga kuli Yehova . ³⁶ Apo Sauli anati , "Tiyeni kwapepeke ma Philisiti usiku nakuwapoka vinthu mpaka kuseni , tisasiyepo uliyonse wamoyo . Wanayankha , "Chitani chilichonse chamene muwona bwino kwa imwe ." Koma wansembe anati , "Tiyeni tifique kwa Mulungu pano." ³⁷ Sauli ana funsa Mulungu , "Kodi ine mwa pitikise ma Philisiti ? Kodi muzawapasa mumanja mwa Israeli ?" Koma Mulungu sas muyankhe kanthu kali konse ija siku. ³⁸ Apo Sauli anati , "Bwelani kuno , imwe wonse azisogoleli wa wanthu ; phunzilani ndipo yang'anani mwamene yachitikila iyi chimo lelo. ³⁹ Pakuti , malingana anapuluma Israeli , olo kuti nimwa Jonathani mwana wanga , uyo azafa vazooni." Koma panali mwa amuna onse pakati pawanthu wamene anamuyankha . ⁴⁰ Ndipo anati kuli Israeli eli yonse , "Mufunika kuyimilila kumbali imozi , ndipo ine na Jonathani mwana tizankhala ku mbali inangu ." Banthu anati kuli Sauli ."Chita chamene chioneka bwino kwa iwe ." ⁴¹ Sauli anati , " Yehova , Mulungu wa Israeli ! Ngati iyi chimo yachitiwa na ine kapena ni mwana wanga Jonathani , nishi , Yehova Mulungu wa Israeli , pelekani yankho pali ichi chotizungulula mitu . Koma ngati iyi chimo yapalamwidwa na banthu wanu a Israeli , pelekani thumiminu ." Apo Jonathani na Sauli anasankhila na mayele , koma asilikali wankhondo wanaziwika kuti wanalibe mulandu. ⁴² Ndipo Sauli anati , "Chitani mayele yolotele pakuti pa ine na mwana wanga Jonathani , " Koma Jonathani anasankhiwa na mayele. ⁴³ Ndipo Sauli anati kwa Jonathani , " Niuze chamene wachita Jonathani anamuwiza " nalawa tu uchi tung'ono nakansonga ka ndodo yamene inali mumanja mwanga . Nilipo pano nizafa." ⁴⁴ Sauli anati , " Mulungu achite icho ndipo achite ichi maningi kuli ine , ngati siuzafa Jonathani." ⁴⁵ Apo banthu wanakamba kuli Sauli kuti , " Angafe Jonathani , wamene alengesa kuti uku kugonjesa kukulu maningi kwa Israeli kukwanilisidwe ? Nchapatali ! Malingana Yehova niwa moyo , olo sisi imozi kuchoka mumutu mwake siyizagwa pansi , pakuti asewenzana na Mulungu lelo. " Ndipo banthu wana leselela Jonathani kwakuti sianafe. ⁴⁶ Apo Sauli analekeza kupitilisa a Philisiti , ndipo a Philisiti anayenda kumalo kwao. ⁴⁷ Pamene Sauli anayamba kulamulila mu Israeli , anamenyana mosusana na wadani kuchokela kumbali zonse - zonse . Anachayana na a Mobu , na Amoniye , Edomu , mafumu waku Zawa , na ma Philisiti . Kuli konse kwamene anatembenikila , anawalasa chilango weve. ⁴⁸ Anachita molimbika mutima maningi nakugonjesa ma Amaleki . Analeselela Israeli kuchoka mumanja mwa waja wamene wanali kumubela katundu muchita nkondo kuli eve. ⁴⁹ Bana ba Sauli wanali Jonathani , Ishvili , na Maliki - Shuwa . Mazina ya bana bake wakazi wabili anali Merabu , woyamba kubadwa , na Michale , mung'ono. ⁵⁰ Zina yamukazi wa Sauli inali Ahinowemu : anali mwana mukazi wa Ahimaazi . Zina ya kapitawo wa masoja wake inali Abinala mwana wa Nala malume wake wa Sauli. ⁵¹ Kishi ndiye anali tate wake Sauli ; ndi Nala , tate wake Abinala , anali mwana wa Abiele . ⁵² Kunali ku menyana zolimba mosusana na a Philisiti masiku yonse ya Sauli . Apo Sauli akaona munthu wamphamvu aliyense kapena akaona munthu aliyense wochenjela wolimbika mtima ndipo wamphamvu , anali kumunyengelele kuti ankhale kugulu yake eve.

Chapter 15

¹ Samueli anati kuli Sauli , "Yehova anatuma ine kukuzoza ufumu pa banthu bake Israeli . Manje mvela mau ya Yehova . ² Ichi ndiye chamene Yehova wamakhamu anena , ' Nasunga mumutima mwanga chamene Ameleki anachita kuli Israeli pakuwa lesa njra nthawi yamene wanachokela ku Egypti . ³ Manje yenda nakunuyamba nkondo Ameleki nakuwanongelatu pasasiyako kanthu zinthu zonse zamene walinazo . Osawasiyako , koma payani wabili bonse wamuna nabakazi , mwana naka cheche , ng'ombe na nkhoa , ngamila na mudoke . " ⁴ Sauli anasonkhanisa banthu nakuwawawelengela pamuzinda wa Telayimu - twu handeledi sauzande wanthu woyenda pansu na Teni sauzande amuna aku ludeya . ⁵ Apa Sauli anabwela kumuzinda wa Amaleki nakuyembekeza mu vale . ⁶ Nipo Sauli anati kuli mo kenayiti . " Yendani chokani , fumani moni pakati pa wa Ameliki pakuti ine nisaku onongeleni pamozi nawo . Pakuti munaonesa chifundo kuli bathu bonse waku Isreali , pamene wanachokela ku Egypti . " Mwa ichi makananayiti wana fendela kutali kuchoka pama Amaleki . ⁷ Ndipo Sauli anawayamba nkondo ma Ameleki kuchokela ku Havila mpaka ku Shuwa , yamene ili chakumumawa kwa Egypti . ⁸ Ndipo anatenga Agagi mfumu ya Ameleki ali wamoyo ; anawonongelatu ko sasiyako banthu wonse na nsonga ya panga . ⁹ Koma Sauli na banthu wanalekelela Agagi pamozi naviweto vabwino maningi vonse , monga ng'ombe , nkhoa , kuyikapo na toyina tuwana twa ng'ombe na nkhoa . Vonse vamene vinali vabwino sibonaviononge . koma banaononga chili chonse chamene sichinali bwino na kuti chinalibe nchito . ¹⁰ Ndipo mau yamulungu yanabwela kuli Samueli , kuti , ¹¹ "Chinikalipo kuti ninankhazikisa Sauli kunkhala mfumu , pakuti akoneka misongo kuchoka kukonkha ine , ndipo sanachite malamulo yanga . " Samueli anakwiya ; analila usiku wonse mokuwa kwa Yehova . ¹² Samueli anauka kuseni seni kuti akumane na Sauli m'mawa . Samueli anauziwa , "Sauli anabwela anabwela anabwela ku Carmeli na ku nkhozika chowumba cha yeve mwine wake , nakukoneka nakupitiliza ulendo kuselukila ku Giligali . " ¹³ Apo Samueli anbwela kwa Sauli , ndipo Sauli anati kwa yeve , " Odalisika ndiwe wa Yehova ! Nakwanilisa chilamulo cha Yehova . " ¹⁴ Smueli anafunsa , "Nanga nichani kuuluma kwa nkhoa mumutu mwanga , makulila kobangula kwa ng'ombe kwamene nimvela?" ¹⁵ Sauli anayankha , " Wavichosa kuli ma Ameleki . pakuti banthu wanasiyapo vabwino maningi pa pankhoa na ng'ombe , kuti avipeleke nsembe kwa Yehova Mulungu wako . Vosala taonongelatu . " ¹⁶ Apo Samueli anati kwa Sauli , " Yembekeza ndipo ine nizakuwuzza zamene akamba kwa ine usiku walelo " Sauli anati kuli yeve , "kamba!" ¹⁷ Samueli anati , " Loko ndiwe mung'ono ukaziona , siunapangiwe mutu wa mitundu ya Israeli ? Ndipo Yehova anakuzoza mfumu pali Israeli yonse , ¹⁸ ndipo Yehova anakutumani kwanu kunena kuti , ' Yenda nakuonongelatu osasiyako wochimwa , ma Amaleki , ndipo umenyane nao mpaka wawonongekelatu . ' ¹⁹ Nichi fukwa chabwanji chamene chalengesa kusamvela liwu ya Mulungu , koma m'malo mwake imwe mwatenga mopanda lamulo na kuchita choyipa mumenso mwa Yehova ? " ²⁰ Apo Sauli anati kwa Samueli , "Ine ninamvela zooni mau ya Yehova , ndipo ninayenda munjila yamene yawe ananituma . Ninamuleta mogwilila mwachikamizo Agiga , mfumu ya Amaleki , ndipo ninawaononga mosasiyako ma Amaleki wonse . ²¹ Koma bathu wanatengako vinangu mwa voshukiliwa pankhondo - nkhoa na ng'ombe , vabwino maningi pavinthu vonse vamene venzo funikila kuwonongeka , kuti tipeleke nsembe kwa Yehova Mulungu wako ku Giligali . " ²² Samueli anayankha , " Kodi Mulungu amakondwela nazo maningi zopeleka zoshoka na nsembe , kulinganizana na kumvela mawu ake? Kumvela nikwa bwino maningi kuchila nsembe , ndipo kumvesesa nikwabwino maningi kupambana ma futa ambelele zimuna . ²³ Pakuti kuukila kulingana nachimo yachita matsenga , ndipo kusaweluzika kuli monga uchimo wa uchipondo . Chifukwa wakana mau ya Yehova , nayeve akukana iwe kunkhala mfumu . " ²⁴ Apo Sauli anati kwa Samueli , "Nachimwa ; pakuti napwanya lamulo ya Yehova na mau yanu , chifukwa ninayopa banthu nakumvelela mau yawo . ²⁵ Manje , napapata khulukani chimo yanga , ndipo mubwelele na ine pakuti ningapembeze Yehova . " ²⁶ Samueli anati kuli Sauli , " Sinizabwelela na iwe ; ndaba wakana mau ya Yehova , ndipo Yehova akukana kuti siuzankhala mfumu ya Israeli . " ²⁷ Pamene Samueli anapiliuka kuti azi yenda , Sauli ana fwemba mupelela mukhanjo wake ndipo nkhanjo wa Samueli unang'ambika . ²⁸ Samueli anati eve , " Mulungu anyonsolako ufumu wa Israeli kuchoka kuli iwe lelo nakuupeleka kuli munthu wamene unkhala naye pafupi , yeve maningi kuchila iwe . ²⁹ Chinangu , mphamvu ya Israeli sazanama kapena kuchinja nzeli zake ; ndaba yeve simunthu , pakuti angachinje uzeli zake . " ³⁰ Apo anati , "Nachimwa . Koma chonde nipaseni ulemu pamenso pa azisogoleli wa wanthu wanga na pamenso pa Israeli . Bwelelani futi na ine , kuti nikapemphele Yehova mulungu wanu . " ³¹ Apo Samueli anabwelela kukonkha futi Sauli , ndipo Sauli anapembeza Yehova . ³² Ndipo Samueli anati Muleteni Agagi mfumu ya Amaleki pano pali ine . " Agagi anabwela kwa iye aliomangiwa ma chaini nakunena kuti , " Zooni kukwinyilila kwa imfa kwa pita . " ³³ Samueli anayankha kuti , " Monga mwamene lupanga yako ya pangisa azimayi kwakhala alibe bana ndiye mwamene awayi wako wazankhalilila bamayi wako walibe mwana pakuti pa bazimayi . " Apo Samueli anajuwa Agagi mumagawo mumenso mwa Yehova ku Giligali .

³⁴ Samueli anayenda ku Ramah , ndipo Sauli anayenda kukwela kunyumba kwake ku Gibeya ya ya Sauli. ³⁵ Samueli sanamu onepo Sauli mpaka siku yakufa kwake chifukwa analila malilo ya Sauli . Mulungu anakwinyilila kuti yeve enze anakhazikisa Sauli kunkhala mfumu ya Israeli.

Chapter 16

¹ Yehova anati kuli Samueli , "uzalila mpaka liti , pali Sauli , kuchokela pamene ine ninamukana kuti ankhale mfumu ya Israeli ? Thila mafuta yazule munyanga yako ndipo uyende . Nizakutuma kwa Jessi waku Bethelumu , pakuti nazisankhila neka m'mozi mwa bana bake bamuna kuti ankhale mfumu yanga." ² Samueli anati , "Nizayenda bwanji? Ngati Sauli azamvela azanipaya ." Yehova anati tenga kang'ombe kakazi uyende nako ndipo ukanene kuti nabwela kupelaka nsembe kwa Yehova . ³ Umuyitane kunsembe ndipo ine nizakuonesha vamene uzachita . Uzafunika kinizozelako wamene nizakawonesa. ⁴ Samueli anachita monga mwamene Yehova anamuuzila nakuyenda ku Bethelhemu. Akulu osogolela muzinda wanabwela kumu kunanya ninshi wanjena na kukamba kuti , " Kodi mwabwela mwamutendele?" ⁵ Anati , "Mumutendele ; nabwela kupeleka nsembe kwa Yehova . Konzekani muziyike podela mweka ndipo mubwele naine kunsembe ." Ndipo anapatula padela Jessi na bana wake wamuna nakuwayitana kunsembe. ⁶ Pamene wanabwela anaona Eliabu nakuzikambisa yeka kuti wozozedwa wa Yehova anali anaimilila pafupi mnayeve . ⁷ Koma Yehova anati kuli Samueli , " Osayangana maonekedwe yake yapanja , kapena pa katalimphidwe ka thupi yake ; pakuti ine namukana . Chifukwa Mulungu saona mwamene munthu aonela ; munthu anayang'ana pa kaonekedwe kapanja ; koma Yehova amayang'ana mmumutima ." ⁸ Apo Jessi anayitana Abinadabu nakumupitisa pamene pa Samueli , ndipo Samueli anati , " Nayeve uyu sasasankhiwe na Yehova." ⁹ Chokonkhapo Jessi anavomeleza Shamma kubwela kupita pali Samueli , koma Samueli anati , " Nayeve uyu Yehova sanamusankhe . ¹⁰ Jessi anapita pamene pa Samueli wana wamuna wokwana Seveni . Pasogolo pake Samueli anakamba kuti , " Yehova sana sankhepo aliyense pali awa." ¹¹ Apo Samueli anati Jessi , " Kushe wonse wana wako wamuna bali pano ?" Eve anayankha , " Kwasala m'mozi koma ndiye mung'ono maningi pali wonse . Koma ayenda kudyesa nkhusa ." Samueli anati kuli Jessi , "Tumani ndipo kamutengeni ; chifukwa sitizankhala pansu mpaka afike pano . " ¹² Jessi anatuma nakumubwelesa . Apa uyu munyamata analiwosazikanza bwino ndipo anali na menso yabwino na maonekedwe abwino maningi . Yehova anati , " Nyamuka , umuzoze ; pakuti niwame uyu." ¹³ Apo Samueli anatenga nyanga yamafuta na kumuzoza pakati pa azibala wake . Muzimu wa Yehova unamukantha namphamvu Davide kuchokela ija siku mpaka pasogolo pake . Apo Samueli ananyamuka nakuyenda ku Rama. ¹⁴ Apa muzina wa Yehova unachoka muli Sauli , ndipo muzina woyipa wotumina na Yehova unamuvuta m'malo mwake. ¹⁵ Anchito a Sauli anati kuli eve , " Onani, muzimu woyipa wotumiwa na Mulungu ukuvuta . ¹⁶ Lekani ambuye wathu mulamulile akapolo wanu wamene wali pali imwe kuti wakasakile munthu wamene ni kaswili pakuyimba chisulo cha harpu . Ndipo pamene muzimu wankhona watumiwa na Mulungu uzabwela pali imwe , yeve azayimba harpu ndipo imwe muzankhala bwino." ¹⁷ Sauli anati kuli wanchito wake , " Nisakilileni munthu wamene angayimbe bwino ndipo mumulete kuno kuli ine. ¹⁸ Ndipo m'mozi wa anyamata ang'ono anayankha , kuti "Ninaonapo mwana wa Jessi mu Bethelhemayiti , wamene na buso pakayimbidwe wolimba , munthu alibe mantha , nimunthu wankhondo , m'mozi wochenjela kakambidwe , mwamuna wokongola ; ndipo Mulungu alinayeve." ¹⁹ Nchifukwa chake Sauli anatuma nthumi kuli Jessi , nakunena kuti , nitumizilenu ine mwana wanu Davide wamene na nkhusa." ²⁰ Jessi anatenga donke wonyamula buledi , chikapu cha wayini , nakambuzi kang'ono nakuvitumiza pamozi na mwana wake Davide kuli Sauli. ²¹ Nipo Davide anabwela kuli Sauli nakungena nchito yake Sauli anamukonda maningi , ndipo anasanduka wonyamula Zida zankhondo za Sauli. ²² Sauli anatuma kuli Jessi , uthenga wokamba kuti , "Muloleni Davide aziyimilila pali ine , pakuti eve wapeza chikondi mumenso mwanga ." ²³ Nthawi zonse muzimu wankhanza ukankhala pali Sauli , Davide anatenga chisulo choyimbila cha harpu nakuliza . Apo Sauli anali kubwelelamo mum'tendele mumutima mwake , ndipo muzimu woyipa unali kuchokamo nakumusiya eve.

Chapter 17

¹ Manje wa Philisiti anakolonganika magulu yawo ya ankhondo kuti wakamenyane . Wanakumanilana pa Sokohu , yamene ili ku yuda wanali watamanga misasa yawo pakati pa Sokohu na Azekaha , mu Ephesi Damulimi. ² Sauli na amuna aku Israeli wanamanga misasa yawo mu vale yaku Elahu naku lemba muzele wankhondo kuti akumane na ma Philisiti. ³ A Philisti anayimilila kumbali imozi pa lupili ndipo Israeli anayimilila pa lupilin kumbali inangu na vale yenze pakati pawo. ⁴ Mwamuna wamphamvu anatulukila kuchokela mu musasa wa ma Philisiti zina yake Goliyade sikisi mipimo na kolundapo . ⁵ Anali na chisote chapangwa na malata pa mutu pake , ndipo anavala chikhoti chankhondo chopangiwa natumalata . Chikhoti chinalema fayivi sauzande masikelo ya mwala wa bulonzi. ⁶ Anali na za bulonzi m'mendo mwake mikondo wa bulonzi munkwapa mwake . ⁷ Ndodo yogwirilako mukondo wake inali yikulu nakanthambo ka kotoni kaponyelako manga mwamene wankhalila kotoni ku chasokelako. Mutu wa nkhondo wake unalemela sikisi handeledi ma shekelo ya chisulo , womunyamulila chozichingilizilako anatangilako pasogolo. ⁸ Anayimilila wakukuwilila pamene panali a Israeli mumisasa yawo , "Mwabwelele chani kutanthama kuti timenyane ? Kodi ine sindine mu Philisiti nanga imwe sindimwe akapolo wa Sauli ? Zisankhileni muthu mweka ndipo mulekeni aseluke abwele kunu kuli ine . ⁹ Ngati angakwanise kumenyana nakunipaya nishi ise tizankhala akapolo wanu. Koma ngati nizamugonjesa nakumupaya , nishi imwe muzankhala akapolo wanthu nakutisewenzela . ¹⁰ Nafuti uja mu Philisiti anati , " Nisusana na mandindo wa Israeli lelo . Nipaseni munthu kuti Aimenyane naye." ¹¹ Pamene Sauli na Israeli yonse inamvela chamene Muphilisiti anakamba , wanamvela ulesi nakuyopa maningi. ¹² Manje Davide anali mwana wa mu Ephrathiti waku Betelehemu mu yudeya wamene ziwa yake anali Jessi. Anali na bana wali eyiti wamuna . Jessi anali munthu wokalamba mumasiku ya Sauli , anali nkhalamba maningi pakati pa wamuna . ¹³ Watatu wakulu maningi wana wa Jessi anali watakonkha Sauli konkhondo . Mazina ya bana wake watatu wamene wanayenda kunkhondo anali Elibu woyamba kubadwa , wachiwili kuli eve ni Abinadabu , ndipo wachitatu anali Shamma. ¹⁴ Davide ndiye anali mung'ono maningi Batatu wakulu maningi wana konkha Sauli kunkhondo . ¹⁵ Apo Davide anali kuyenda yenda uku na uku pakati pa gulu ya ankhondo wa Sauli na nkhosa na atate ku Betelehemu pakuti aziwadyesa . ¹⁶ Kwa masiku tote munthu wamphamvu wa a Philisiti anali kubwela pafupi na mumawa na mumazulukuzipoteke yeka kuti wamenyane. ¹⁷ Apa Jessi anati kuli mwana wake Davide , "Peleka kwaazibale wa ko efa imozi ya Nshawa na yiwaya vokazinga , na aya mikhate yali teni , nakuvipeleka musanga kuli azibale wako. ¹⁸ Nafuti upeleke ivi vakudya vamkaka vili teni kuli kapitawo wawo , uja sogolela asilikali sauzande . Uwone mwamene alili azibale wako ndipo uleteko kuno umboni walkuti wali chabe bwino. ¹⁹ Azibale wako wali na Sauli na bamuna wonse wanu Isreali mu vale ya ku Elaha, wamenyana nama Philisiti." ²⁰ Davide anauka m'mamawa nakusiya viweto mumanja mwa nchiweta . Anatenga vopeleka nakuchoka , monga chabe mwamene Jessi anamulamulila eve. Anabwela mu kampu panthawi yamene asilikli wanali kuyenda kamuzele wo menyanilanapo alikuliza belu yankhondo. ²¹ Ndipo Israeli na asilikali wa a Philisiti wanatanthamila kumenyana , gulu ya asilikali kumenyana na gulu ya asilikali. ²² Davide anasiya vatundu wake kuli wosunga votumizidwa , anathamangila gulu ya wankhondo , nakuposhana na azibale wake. ²³ Pamene anali kukamba nawo , mwamuna wamphamvu , mu Philisiti waku Gathi , Goliade zina yake , ndipo anatulukila kuchoka kumbali ya a Philisiti , na kuncha mau yamozi na yamozi monga poyambilila , na Davidde anayamvela . ²⁴ Pamene onse amuna aku Israeli banaona uyu munthu ,wana thawa kuchoka kwe anali ndipo anachita mantha maningi. ²⁵ Amuna aku Israeli anati mwamuona uyu munthu wamene wayimilila ? Abwela kumushusha Israeli . Mfumu izapasa chuma chambili kuli munthu wamene azamupaya , nakupasa mwana wake mkazi kuli uyu munthu kuti amukwatile , ndipo azachitisa nyumba ya batate wake owasuliwa kuleka kupeleka musonkho mu Israeli. ²⁶ Davide anati kuli azimuna wamene anyimilila pafupi naye , "Nichani chizachitika kuli munthu wamene azapaya uyu mu Philisiti nakuchosa manyazi pali Israeli ? Ndani uyu mu Philisitini wasadulidwa kuti azi delela magulu ankhondo a Yehova wa moyo?" ²⁷ Banthu wanabwezapo vamele analikukamba nakuwuzwa kuti , " Va chancha ndiye vamele vizachitika kuli munthu wamene azapaya uyu Philisiti . " ²⁸ Eliabu mukulu maningi pa nzikulu wake monse analimwela pamene Davide anali kukamba na waja banthu . Ukali wa Eliabu unabuka kukwiyila Davide , ndipo anati , " Wabwelele chani kuno? " Wasiyila ndani tuviweto tung'ono tuja musanga ? Niziwa chimeko chako , nazochita zosotongosoka zamumutima mwako ; pakuti watelemukila kuno pakuti uone kumenyana . " ²⁹ Davide anati , "Nachita chani manje ? siinali funso chabe?" ³⁰ Ana piliwukila winangu, nakukamba munjila imozi na imozi. Banthu wanayankha vinthu vimozi monga nipoyamba. ³¹ Pamene mau yamene Davide anakamba yanamveka, masoja anayabwezapo kuli Sauli , ndipo anatuma nthumi kumuitana Davide. ³² Ndipo Davide anati kuli Sauli , "Mtima wa munthu aliyonse usakomoke chifukwa cha mu Philisiti uyu ; apolo wana nizayenda na kumenyana na mu Philisiti uyu. " ³³ Sauli anati kuli Davide , " Siungakwanise kuyenda

kushushana na uyu nu Philisiti loko kumenyana naye ; chifukwa ndiwe chabe munyamata , koma eve ni munthu wankhondo kuchokela ku ufana wake." ³⁴ Koma Davide anati kuli Sauli , " Kapolo wanu ninalikusonga nkhusa za atate wanga . Pamene mkango nangu beya vinalikubwela na kugwilapo kamwana kankhusa kuchosa paviweto, ³⁵ ninali ku chipilikisa na kuchimenya , naku kapulumusa kukachosa mukamwa mwake . Chinyama chifa chikaunkila ine , ninali kuchigwila ndevu , kuchimenya , nakuchipaya." ³⁶ Kapolo wanu nipayapo kudala vonse vibili mkango na beya uyu mu Philisiti wosaduliwa aza sanduka monga m'mozi wa ivi vinyama ve nakambapo , pakuti ayambana na magulu ya ankhondo a Yehova wamoyo." ³⁷ Davide anati , " Yehova ananileselela ine kunichosa kukwando kwake kokabawula kwa nkhalamu na kwa beya . Azanileselela kunichosa mukwanja kwa uyu muPhilisitina. " Apo Sauli anati kuli Davide , venda , ndipo Yehova ankhale na iwe." ³⁸ Sauli anavalika Davide zida zake za nkondo . Anayika chisote chamalata ya bulonzi pamutu pake , ndipo anamuvalika chikhoti chopangiwa na tumalata tung'ono tung'ono. ³⁹ Davide anasomeka lupanga yake muli ivi vovala vankhondo . Koma sanakwanise kuyenda chifukwa sianachite navo chikonzekelo . Apo Davide anati kuli Sauli , siningayende kunkhondo na ivi pakuti sinanakonzekele naveve ." Choncho Davide anavi vula nija vevala vankhondo. ⁴⁰ Anatenga ndodo yake mumanja nakudoba tumyala tuli fiyivi kuchoka mukamufolo kamene kamapeleka manzi kukamawa ku kulu . nakuyayika mukachola kamuchiweta . Malegeni yake yenze mumanja pamene anafika pafupi na mu Philisitina. ⁴¹ Mu Philisitina anbwela nakupalamilana na Davide , apo wonyamula chishongo wake ali pasogolo pake. ⁴² Pamene mu Philisitina anayangana pozunguluka nakuwona Davide , anamusula ndaba anali m 'nyamata chabe , ndipo wamonekedwe akongola ndi yowala na yosweta. ⁴³ Apo mu Philisitina anati kuli Davide , " Kodi ndine galu , pakuti ubwele kuli ine na mitengo ? " , ndipo mu Philisitina anatembelela Davide kusewenzesa milangu ya kwao. ⁴⁴ Mu Philisiti anati kuli Davide , " Bwela kuli ine ndipo nizapasa nyama yako kuvinyoni va mumwamba nakuvinyama vamusanga ." ⁴⁵ Davide anayankha mu Philisitina kuti , " Iwe wabwela kuli ine na panga , mkondo , nacholasilako chamutengo . Koma ine nibwela kuli iwe muzina ya yehova wamakhamu , Mulunu wa magulu ankhondo aku Israeli wamene wanyoza. ⁴⁶ Lelo Yehova azanipasa ine kupambana pali iwe ndipo nizakupaya iwe nakukufuwa mutu kushosa kuthupi yako . Lelo ine niza pasa mitembo yama Philisitina vinyama vamusanga , pakuti , ziko yapansi yonse izaziwa kuti kuli Mulungu mu Israeli, ⁴⁷ ndipo kuti musonkhano wonse uyu uziwe kuti Yehova sapasa chigonjeso kupitila muli mapanga na mikondo . Pakuti nkondo niya Yehova ndipo azakupasani mumanja mwathu." ⁴⁸ Pamene mu Philisitina ananyamuka nakufendela pafupi na Davide ,apo Davide anathamanga mwamusanga kuyenda kuli gulu yankhondo ya adani kuti akumane naye. ⁴⁹ Davide anangenesa kwanja yake mukachola kake , anachosamokamwala kosalala, anakazungulusa komangilila kunthambo nakukaponya kwa Goliade pamphumi , ndipo anagwa choyang'ana nkhope yake pansi. ⁵⁰ Davide anagonjesa mu Philisiti naka nthambo na mwala anachaya mu Philisiti na kumupaya . Munalibe panga mumanja mwa Davide. ⁵¹ Apo Danide anathamanga nakukwela pa mu Philisiti nakutenga panga yake , nakuisolola kunja kwa chikwama chake , nakupaya ene , nakumujuwa nacho mutu . Pamene Aphilisiti anaona kuti munthu wao wamphamvu wafa wanathawa. ⁵² Ndipo banthu waku Israeli na Yudeya wananyamuka nakupunda , nakupilikisa mumambuyo mwa ma Philisiti mpaka kufikisana ku vale namageti yaku Ekiloni . Ma Philisiti wokufa wanagona mumbali mwa njila yoyenda ku Shaaraimu , njila yonse yaku Gathi na Ekroni. ⁵³ Bathu waku Isreli wanabwelela ku chokela mukupepeka ma Philisiti ndipo wanapoka vinthu venzeli mu misasa yawo. ⁵⁴ Davide ananyamula mutu wa mu Philisiti nakuwubwelesa ku Yelusalemu , koma anaika zida zankhondo zamu Philisiti kutenti yake eve Davide. ⁵⁵ Pamene Sauli anaona Davide ayenda kunja kukamenyana na mu Philisiti , anati kuli Abinala kapitawo wa a nkondo , " Abinala mwana wandani uyu munyamata ? " Abinala anayankha , " Malinga mulona moyo , mfumu ine siniziwa." ⁵⁶ Mfumu inakamba kuti , " Funsu kuli waja wamene wangaziwe , kuti m'nyamata ni mwana wandani ." ⁵⁷ Pamene Davide anabwelela kuchokela mkupaya mu Philisiti , Abinala anamutenga naku mubwelesa kuli Sauli na Mutu wa mu Philisiti mumanja mwake . ⁵⁸ Sauli anati kuli eve , " Ndiwe mwana wa ndani , iwe m'nyamata mufana? Davide anayankha , " Ndine mwana wa kapolo wanu Jessi mu Bethlehemayiti."

Chapter 18

¹ Pamene anasiliza kukamba na Sauli moyo wa Jonathani unamangilika kuli moyo wa Davide , ndipo Jonathani anamukonda monga mwamene akondela moyo wake. ² Sauli anatenga Davide kuti azimusewenzela ; sanamulole kubwelela kunyumba kuli watate wake. ³ Ndipo Jonathani na Davide anapangana chipangano cha ubwenzi chifukwa Jonathani anamukonda monga nimoyo wake chayiwo. ⁴ Jonathani anvula chinkhanjo chamene enzeli vale nakuchipasa kuli Davide na zovala zake zankhondo , pamozi na panga yake , utha, na beluti. ⁵ Davide anali kuyenda kuli konse Sauli akamutuma , ndipo anakukwanilisa . Sauli anali kumutuma kusogolela wanthu wankhondo . Ichi chinakondwela banthu wonse wamene wanachiwona ndiponso mu manso mwa wanchito wa Sauli. ⁶ Pamene wanali kubwela kunyumba kuchokela kugonjesa ma Philisiti , azimayi wanabwela kuchokela kumizinda yonse ya Israeli apo wayimbanakuvina kuti akumane na mfumu Sauli , namatambolini , nachikondwelelo na zisulo zamayimbidwe. ⁷ Azimayi anali kuyimbilana winangu kuli munzake apo wasowela . Wanali kuyimba kuti: " Sauli anapaya masausande wake , koma naye Davide ma teni sausande wake." ⁸ Sauli analemiya maningi , ndipo iyi nyimbo inamuchima . Anati , " Wazipelekela ulemu wama teni sausande kuli Davide koma kuli ine ulemu wa sausande chabe . Nichani chinangu chamene chasalako kumupasa , pakuti kwasala chabe ufumu?" ⁹ Sauli anali kuyang'ana Davide namutima wachikayiko kuchokela iyo siku kuyenda pasogolo. ¹⁰ Siku inakonkhapo muzimu wankhonza unamukuntha sauli ndipo anayenda yenda munyumba . Apo Davide analiza chilimba chake , mwamene anali kuchitila siku iliyonse . Sauli anali m'kondo mumanja mwake. ¹¹ Apo Sauli anaponya mukondo chifukwa anaganiza kuti , " Nizamuphinila Davide kuchiwumba ." Koma Davide anathawa kuli Sauli kabili muli uyu musango. ¹² Sauli anachita mantha kuyopa Davide , chifukwa Yehova anali naye , koma sanalinso na Sauli. ¹³ Nchifukwa chake Sauli anamuchosa m'manso mwake nakumusankha nkulu wa gulu ya Davide khonko wali sauzande. Mwanjila iyi Davide anali kuchoka nakubwelela alikusogolela banthu. ¹⁴ Davide anali kutukuka mu njila zake zonse pakuti Yehova anali naye. ¹⁵ Pamene Sauli anaona kuti anatumuka , ananyamuka mukundabwa kwa mantha . ¹⁶ Koma Israeli yonse na Yudeya wana mukonda Davide , chifukwa analikuwa sogolela poyenda napo bwela . ¹⁷ Ndipo Sauli anati kuli Davide , " Uyu mwana wanga mukulu pawonse marabu , nizamupasa kuli iwe kuti ankhale mukazi wako. Chabe ankhale wozipeleka wanga nakumenya nkhondo za Yehova ." Pakuti Sauli anaganiza kwanja kwanga kusankhale pali eve , koma lekani manja yama Philisiti ndiye yakamupaya." ¹⁸ Davide anati kwa Sauli , "Ndine ndani , na wa bululu wanga niwandani loko chiwongo chawa dadi mu Israeli , pakuti nipezeke mpongozi wazooni wa mfumu?" ¹⁹ Pali ija nthawi pamene merabu , mwana wa Sauli , anali kwenekela kupasiwa kuli Davide , anapasiwa kuli Adriele mu Metholathiti kunkhala mukazi wake. ²⁰ Koma Michalu mwana wa Sauli , anakonda Davide wanamuuza Sauli ndipo ichi chunamu kondwelesa iye. ²¹ Apo Sauli anaganza , "Nizamupasa kuli eve, pakuti ankhale nyambo yomukashilako na kuti kwanja kwa a Philisiti kunkhale mosusana naye . Apo Sauli anali kuli Davide ka chibili , " Iwe uzankhala mpongozi wanga." ²² Sauli analamulila wanchiyo wake , "Kamba naye Davide payeka ndipo ukambe kuti, ona mfumu yakondwela na iwe , ndipo wonse wanchito wake akukonda , manje apa nkhal mpongozi wa a mfumu." ²³ Apo wanchito wa Sauli anakamba aya mau kuli Davide . Ndipo Davide anati , "Myesa nichinthu chapafupi kwa iwe kunkhala mpongozi wa mfumu , pakuti nine munthu wosauka , na wosawelengelewa?" ²⁴ Wanchito wa Sauli anamuuza anamubwezela uthenga wa zimene anayankha Davide. ²⁵ Apo Sauli anati , " Mukambe ichi kuli Davide , ' Mfumu siyi funa kuti mulipile vilivonse pali mukazi kupafulapo chabe nkanda za pamensozili handeledi zama Philisiti , pakuti mfumu anaichitila .'" Apa Sauli anaganiza kuti apayise Davide kupitila mukwanja kwa ma Philisiti. ²⁶ Pamene wanchito wake wanauza Davide aya mau , china mukondwelesa Davide kuti ankhale mpongozi mwamuna wa mfumu. ²⁷ Akalibe kukwanili aja masiku , Davide anayenda na masoja wake nakupaya ma Philisiti yali thwu handeledi , Davide abwelesa nkanda zawo zapamenso , ndipo wanazipeleka numbala yokwana mwamuna wa mfumu . Ndipo Sauli anamupasa Michala mwana wake kuti ankhale mkazi wake. ²⁸ Pamene Sauli anaona nakuziwa kuti Yehova anali na Davide , na kuti Michala , mwana wa mkazi wa Sauli , anamukanda eve, ²⁹ Sauli anamuyopa kuyikililako maningi Davide . Sauli anasanduka mudani wa Davide kwa muyaya. ³⁰ Chokonkhapo akazembe wa ma Philisiti anatulukila , kunja kunkhondo , ndipo mwamene pafupi pafupi wanali kutulukila , Davide analikupambana maningi kuchila wonse wanchito wa Sauli , kwakuti zina yake inalemekezeka maningi.

Chapter 19

¹ Sauli anati kuli mwana wake Jonathani na kuli wanchito wake wonse kuti wafunika kumupaya Davide . Koma Jonathani , mwana wa Sauli , anali kukondwela maningi na Davide. Nchifukwa chake Jonathani anauza Davide , " Sauli tate wanga afuna kukupaya iwe . ² Nchifukwa chake uchenjele kuseneni ndipo uzibise mumalo osaziwika . ³ Ine nizayenda kunja nakuimilila pafupi na batate wanga munsanga mwamene uzankhala , nakukamba na watate wanga za iwe . Nikayenda kuziwapo vilivonse ine nizakuwuzwa." ⁴ Jonathani anakamba bwino kuli tate wake za Davide nakunena kuti eve kuti , osati mfumu ichimwile kapolo wake Davide . Pakuti sianakulakwilani imwe, ndiponso zichitidwe zake zakuletelani ubwino. ⁵ Pakuti anatenga moyo wake mumanja mwake popaya mu Philisiti . Yehova analeta kuchimfya kukulu kuli Israeli yonse . Munachiona ici nakukondwela maningi.Nchifukwa chani mufuna kuchimwila mwazi wosalakwa po paya Davide kulibe chifukwa?" ⁶ Sauli anali kumuelelela Jonathani . Sauli analapila kuti, " Malingana Yehova niwamoyo , sazapayiwa." ⁷ Apo Jonathani anayitana Davide , ndipo Jonathani anamuwuzwa izi zinthu zonse , Jonathani anabwelesa Davide kuli Sauli , ndipo anali mumenso mwake monga kudala. ⁸ Kunali nkondo futi , ndipo Davide anayenda kunja kukamenyana nama Philisiti nakuwa gonjesa nakuwapaya maningi . Wanamuthawa. ⁹ Muzimu woyipa wotumiziwa na Yehova unabwela pali Sauli pamene anali kunkhala munyumba mwake na mkondo wake mumanja ndipo pamene Davide anali kuliza chisulo chake . ¹⁰ Sauli anayeselela kumuphinila kuchiwumba namukondo Davide , koma anamyomyoloka kuthawa panali Sauli , mwakuti Sauli analasa muchiwumba na ija mkondo . Davide anajumpha nakuthawa uja usiku. ¹¹ Sauli anatuma nthumwi zake kunyumba kwao Davide kumulonda pakuti akamupaye kuseneni . Michala , mkazi wa Davide , anamuwuzwa , "Ngati siupulumusa moyo wako usiku walelo mailo uzapayiwa." ¹² Apo Michala anaselusa Davide kupitila pa windo . Eve anayenda nakuthawa, nakusowa. ¹³ Michala anatenga chikadoli chamunyumba wakuchigoneka pa bedi . Ndipo anayika pillo wa masaka yambuzi kumitu , nakuchiphimbana vovala. ¹⁴ Pamene Sauli anatenga nthumwi kuti zitenge Davide , mkazi wake anati , " Mwodwala." ¹⁵ Apo Sauli anatuma nthumwi zoyenda kumuona Davide ; anati , "Muleteni kuno kuli ine mubedi , pakuti nimupaye." ¹⁶ Pamene anthumwi wanangena mukati , onani ; chikadoli chamunyumba chinaligone pabedi pamozi napillo ya masaka ya mbuzi kumitu kwake . ¹⁷ Sauli anati kuli Michala . "Waninamila chani nakulekelela mudani wanga ayenda , pakuti athawa nakusowa ?" Michala anayankha Sauli , "Anati kuli ine , ' Nileke niyende ufuna nikupayile chani iwe?" ¹⁸ Apo Davide anathamanga nakuthawa , ndipo anayenda kuli Samueli ku Roma na kumuuzwa zonse zamene Sauli anachita kuli eve. Apo eve na Samueli anayenda na kunkhala ku Nayothi. ¹⁹ Chimaenziwa kuli Sauli , kuti , "Onani , Davide aliku Nayothi mu Roma." ²⁰ Apo Sauli anatuma nthumwi kuti akamugwilile Davide . Pamene anaona gulu ya aneneli ili kusesema , ndipo Samueli amilila monga musogoleli wawo , muzimu wa Mulungu unabwela pali waja nthumwi wa Sauli , ndipo naweve wananenera. ²¹ Pamene Sauli anuziwa za ichi, anatuma nthumwi zinangu , ndipo naweve anachita uneneli . Ndipo Sauli anatuma ma nthumwi wenangu gulu yachitatu, naweve futi wanasesema . ²² Ndipo na yeve anayenda ku Roma anakufika chisime chitali chaku Seku . Anafunsa , " Alikuti Smueli na Davide?" Winangu anakamba kuti , "Onani, wali pa Nayothi mu Roma . " ²³ Sauli anayenda ku Nayothi mu Roma.Muzimu wa mulungu unabwela pali eve,ndipo pamene anali kuyenda ananenela mpaka anafika pa Nayothi mu Roma. ²⁴ Anavula mochita kung'amba vovala vake kunenela nayeve mumenso mwa Samueli . Anagona chinthako muzuba monse na usiku wonse . Ichi nichifukwa chake wana funsa " Kushe Sauli anayeve ali m'mozi wa aneneli?"

Chapter 20

¹ Apa Davide anathawa kuchoka ku Nayothi mu Roma nakubwela nakukamba kuli Jonathan,"Nachita chani?" Kusalungama kwanga nikuti? Chimo yanga kuli wa tate wako Riyabwanji, pakuti afuna-funa kutenga moyo wanga?" ² Jonathan anati kuli Davide,"Nchapatali siuzafa.Atate banga siwachita chinthu kapena chikulu kapena ching'ono kulibe kuniuzako ine. Nichifukwa chani watate wanga lwangabise ichi chinthu kuli ine? Simuwamene chili." ³ Kama Davide analapa futi nakukamba ati,Watate wako waziwa bwino kuti ine ninapeza chikondi kuli iwe. Anakamba ati,'Osamuwuza Jonathan za ichi, angakwinyilile!Koma malingama Yehova niwamoyo, ndipo na iwe ulimoyo, pakaliko koma mupata pakati pa ine na imfa," ⁴ Apo Jonathan anati kuli Davide, "chilichonse chamene uzakamba,nizakuchitila iwe." ⁵ Davide anati kwa Jonathan, Mailo ni mwezi wanyowani,ndipo nifunika kunkhala pansi nakudya na Mfumu. Koma leka niyende kuti nikazibise musanga mpaka siku yachitatu mumazulo. ⁶ Ngati atate wako azanifuna m'jila iliyonse,ndipo iwe ukakambekuti,"Davide anapempela liwi molimbikila maningi kuli iwe pakuti angathamangile ku Bethlehemu muzinda wa kwawo; chifukwa nithawi ya nsembe yapa chaka kuja pamukoka wonse. ⁷ Ngati auzakamba kuti chili chabe bwino ninshi kapolo wanu nizankhala namutendele.Koma ngati azakalipa maningi,apo muzaziwa kuti waganizila kuchita choipa. ⁸ Nachifuka chake muchite mwachi fundo na kapolo wanu.Pakuti munangesa kapolo wanu muchipangano cha Yehova naimwe.Koma ngati muli chimo mwa ine,munipaye imwe mwawene;ndaba nchifukwa bwanji ndipo chamene muzaniletela kuli wa tate wanu?" ⁹ Jonathan anati,chinkhale kutali na iwe!Ngati nizaziwa kuti atate wanga wanganiza choyipa kuti chibwele pali iwe,kushe ine siningakuwuze iwe?" ¹⁰ Apo Davide anati kuli Jonathan,"Ndani azaniuza ngati pali mpata wakuti atate wako azayankha mwa ukali maningi?" ¹¹ Joathan anati kuli Davide,"Bwela,tiye tiyende kunja Musanga,"ndipo wonse abili wanayenda Musanga ¹² Jonathan anati kuli Davide,"Yehova Mulungu wa Isaeli ankhole niumboni.Nikayenda kufunsa atate wanga pafupi fupi ino nthawi mayilo,kapena pa siku yachitatu,ona,ngati kuli manganiza abwino pali Davide, ninshi ine simungatume kuli iwe na kuchiulula kuli iwe?" ¹³ Ngati chizakondwelesa atate wanga kuti akuchite choipa,Yehova achite kuli Jonathan namaningi futi ngati siniza chiulula kuli iwe nakukutumiza kutali,pakuti ungayende mumuntendele.Yehova ankhale na iwe,monga mwamene analili na watate. ¹⁴ Ngati nikali namoyo,kuche siuzanionesa ine kukhulupilika kwa chipangano cha Mulungu kuti nisafe?" ¹⁵ Osajuwa ichipangano chanu kukhulupilika kwako kuchokela kju nyumba kwanga kwamuyaya-olo pamene Yehova azajuwa kuchosako wonse wa ndani wa Davide kuchoka paziko yapansi." ¹⁶ Ndipo Jonathan anapanga chipangano na nyumba ya Davide kukamba kuti,"Mulungu afuna kulondolola kuchoka mukwanja kwa adani wa Davide." ¹⁷ Jonathan analengesa Davide alapile futi chifukwa cha chikondi chamene anali nacho pali eve,chifukwa anamukonda mwamene anakondela moyo wake. ¹⁸ Apo Jonathan anati kuli eve,"mayilo ni mwezi wanyowani ,uzayeweka chifukwa mpando wako uzankhala palibe muntu. ¹⁹ Ukayenda kunkhala masiku yatatu,ukatelemuke Musanga nakubwela ku malo yamene wenze unabisamako weka pamene ichi chinthu chofuma kukupaya chenye mumanja,ndipo ukankhale pafupi na mwala Ezel. ²⁰ Nizakaponya tolasila mu uta tutatu kuside kwake,monga nilasa kanthu. ²¹ Ndipo nizatuma munyamata wanga na kunena kuli eve kuti,'yenda utupeze tumivi,' Ngati nizakamba kuli munyamata wamung'ono, 'ona,miviili kumbali iyi yako;yatenga,'ninshi ukabwele;pakuti kuzankhala chitetezo kuli iwe osati choyipa, malingama Mulungu ni wamoyo ²² "Koma ngati nizanena kuli munyamata, 'ona, mivi yali kupitilila pali iwe,ninshi iwe akayende kwanu, pakuti Yehova akutumiza kutali. ²³ Pali chipangano chamene iwe na ine takambilana, ona, Yehova ali pakati pa iwe na ine kwamuyaya.'" ²⁴ Apo Davide anazibisa yeka Musanga.Pamene mwezi wanyowani unankhala,Mfumu inakhala pansi kuti adye chakudya. ²⁵ Mfumu inakhala pamupando wake, monga mwa nthawi zonse, pamupando wamene unali kufupi kachiwumba.Jonathan anayimilila, ndipo Abinala anankhala pafupi kumbali kwa Sauli. Koma mala ya Davide panalibe munthu. ²⁶ Chodabwisa Sauli sanakambepo chinthu chilichonse ija siku,chifukwa ananganiza "chinthu chinangu chamuchitikila.Siwoyela; zoona siwoyera," ²⁷ Koma siku yachiwili, siku yokonkhapo mwezi wanyowani, malo ya Davide panalibe munthu. Sauli anati kuli mwana wake Jonathan ,"nichani mwana wa Jessi sanabwele kuchakudya kapena mailo loko lelo?" ²⁸ Jonathan anamuyankha Sauli kuti, "Davide anapempha molimbika kuli ine kuti ayende ku Bethelumu. ²⁹ Anati ,"chonde lekani niyende. Pakuti Banja yathu iyendo chita nsembe mumuzinda, ndipo mbale wanga wani lamulila kuti nipezekeko. Lomba ngati napeza chifundo kuli imwe, napapata lekani niyende nikaone azibale anga.' nchifukwa chake eve sanabwele ku tebulu yamfumu. ³⁰ Apo ukali wa Sauli unanyeka pali Jonathan, ndipo anati kuli eve, "iwe mwana wa muzimayi wapotozeka, na wowukila! Nanga ine siniziwa kuti iwe unasankha mwana wa Jessi kunsoni zako wemwine, na kumanyazi ya chithanku cha a mai wako?" ³¹ Pakuti malingana mwana wa Jessi ali wamoyo paziko yapansi, kulibe iwe loko ufumu wako. Kutu ukankhazikike.Manje kansi, tuma ndipo umulete kuli ine, ndawa afunika kufa vazoona." ³² Jonathan anayankha atate wake kuti, "Nipali chifukwa bwanji kuti afunika

kupayiwa? Achita chani? ³³ Apo Sauli anamuponyela mkondo wake kuti amupaye. Kamba ka ichi Jonathan anaziwa kuti atate wake analikufunisisa kuti amupaye Davide. ³⁴ Jonathan ananyamuka kuchoka pa tebulo na ukali woyofya ndipo sanadye chakudya pa siku yachibili ya mwezi, Ndawa anankhala na chisoni pali Davide chifukwa atate wake wenze wanamusula eve. ³⁵ Mumawa Jonathani anayenda kusanga monga mwachipangano kumalo anene anapangana na Davide, ndipo munyamata mung'ono anali nayeve. ³⁶ Anati kuli munyamata wake "thamanga upeze mivi yamene naponya" pamene munyamata anali kuthamanga, analosa muvi kumupitilila. ³⁷ Pamene munyamata anafika pamalo pamene muvi wamene anaponya Jonathani unagwela, Jonathani anamuyitana munyamata nakuti kushe muvi siuli kusongola kupitilila pali iwe?" ³⁸ Ndipo Jonathani anayitana munyamata, yendesa, fulumila, osankhalila!" Apo munyamata wa Jonathani ana wonkhesa ija mivi nakubwela kuli Mbuye wake. ³⁹ Koma munyamata sanaziwe vilivonse. Chabe Jonathani na Davide ndiye anaziwa za ichu chisinsi. ⁴⁰ Jonathani anapasa zida zake zankhondo kuli munyamata wake nakukamba kuli eve kuti, "yenda, vipeleke mutawuni," ⁴¹ Nthawi ying'ono ing'ono maningi atayenda miyamota, Davide anayimilila kuchokela kumbuye kwa chulu, anangowa kuyang'ana nkhope yake pansi, nakuwelama yeka katatu. Wanapasana makissi nakulila mokuwa pamozi, analila maningi kuchilapo ni Davide. ⁴² Jonathani anati kuli Davide, yenda muntendele, chifukwa ise tonse tinalapila m'zina ya Yehova, leka Yehova ankhale pakati pa iwe na ine, na pakati pa mbadwa zanga na mbadwa zako, kwamuyaya." Apo Davide anayimilila nakuchoka, ndipo Jonathani anabwela mumuzinda.

Chapter 21

¹ Apo Davide anabwela ku Nobu kuti awone Abimelechi wansembe. Abimelechi anabwela kukumana na Davide apo ali kunjenjemela nakumena kuli eve kuti, "chifukwa pamene muli mweka ndipo palibe wamene muli naye?"

² Davide ananena kuli Abimelechi wansembe kuti, "Mfumu yanituma ku missioni na kunena kuti iwe kuti, asaziwe aliyense za chamene nakulamulila iwe," Natuma anyamata kumalo enangu. ³ Apo manje uli nachani mumanja mwako? nipaseko mikate fayivi ya buledi, Loko vilivonse vamene uli navo kuno," ⁴ Wansembe anayankha Davide kuti, "kulibe mkhate wamba kuno m'mana mwanga koma kuli mkhate woyela-ngati anyamata siwanagone na mkazi asliyonse." ⁵ Davide anayankha wansembe, "Nzoona kuti azimayi sanapasidwe kuli ise kwa masiku atatu yapita, monga mwa nthawi zonse nikanyamuka ulendo. Mathupi ya azibambo yamankhala yopatulika ungankhale niulendo wamba chabe. Nanji lelo paulendo wamutunduyu mathupi ya anyamata yazapatulika mwa mtundu wa bwa!" ⁶ Apo wansembe anamupasa buledi yamene yenze ina ikiwa padela. Pakuti kunalibe bulendi kuja kupatulapo bulendi ya mushilo yamene inachosewa pamensa pa Yehova, Pa chifukwa chakuti akachosapo iyi bulendi abwezelepo buledi yokupya, pasiku yamene ija wanachosapo yozizila. ⁷ Manje mumozi wa chito wa Sauli anali kwamene uku ija siku, osungwa mwachikakanizo ⁸ Davide anati kuli Ahimelechi, "Apo kulibe kuno m'manja mwanu mkondo uliwonse kapena macheti? pakuti sininabwele na panga yanga nangu zida zangu zankhondo pamozi na ine chifukwa nchito yosewenzela amfumu inali lubilo." ⁹ Wansembe anati "Lupanda yo Goliade mu Philisiti wamene unapaya Valle ya Elaha, ilikuno yo pomba mu nyula kumbuyo kwa Ephodi. Ngati ufuna uyitenge, tenge, pakuti kulibe chida chilichonse kuno." Davide anati kulibe Lupanga inangu yamene ija; ipaseni kuli ine." ¹⁰ Davide ananyamuka nakuthawa ija sikukuchoka kuli Sauli nakuyenda kuli Achishi, mfumu ya ku Gathi. ¹¹ Wanchito wa Achish anatikuli eve, "Uyu si Davide, mfumu ya kumalo? kodi sanali kuyimbilana nyimbo za eve povina, Sauli anapaya wake ma sauzande ndipo Davide yake ma teni sauzande?" ¹² Davide anasunga aya mau mumutima ndipo chamuyopa maningi Achish, mfumu yaku Gathi. ¹³ Anachinja misango yake pali weve na kuchita monga wofuutha m'manja mwawo; amalembalemba pa viseko vapageti nakuleka mate yake yakankhulukile pansu kundevu zake. ¹⁴ Apo Achish anati kuli wanchito wake, "chani, muona kuti uyu munthu niwo funtha. Mwamuletela chani kuli ine?" ¹⁵ Kushe nine woshota wanthu wofuntha, pakuti mwaleta uyu munthu wa chabe kuti azichita monga nimumozi wao mumanso mwanga? Kushe uyu munthu wamba angabwele zoona munyumba mwanga?"

Chapter 22

¹ Apo Davide anachokako kuja nakunthawila ku vilindi vamulupili vaku Adullamu. Pamene anazibale wake nawonse waku nyumba kwa atate bake wanavela za ichi wanayendako kwamene analili. ² Aliyense wamene anali kuvutika mumutima, aliyense wamene anali nankhongole, na aliyense wamene sanali wonkhutilawonse wanasonkhona momu zunguluka. Davide anasanduka kapitao wawo. Anali nachiwelengelo chapafupi fupi amuna folo handiledi pamozi naye. ³ Apo Davide anayenda ku Mizipa mu Moabu. Anati kuli mfumu yaku Moabu, "Napapata lekeni atate na amai wanga wayende na imwe mpaka niziwe zamene Mulungu azanichitila." ⁴ Anawa siya kuli mfumu yaku Moabu. Atate wake na wa mai wake wanankhala na eve nthawi yonse yamene Davide anali mumalo yachitetezo chake. ⁵ Ndipo mneneli Gadi anati kuli Davide, "osankhala mumalo yako yachitetezo. choka uyende ku malo ya Yudeya. Apo Davide anachoka nakuyenda musanga yaku Herethi. ⁶ Sauli anavela kuti Davide wapezeka, pamozi na banthu wamene wanelinaye. Apo Sauli anali nakhale mu Gibeya muni mwa mtengo wa tamansiki ku Ramaha, na mkonde m'manja mwake, ndipo wonse wanchito wake waneli yimilile momuzunguluka. ⁷ Sauli anati kuli anchito wake wamene wanayimilila momuzunguluka, 'Mvelani manje, wanthu wa Benjamini ! Kushe mwana wa Jessi azakupasni minda na malo yolimapo mipesa imwe monse? Kushe azakupangani imwe monse akapitawo wa masauzande na makapi tawo wama handiledi, ⁸ Kuti yankhale malipilo yakuti imwe monse mukonzeke chiweubu moukila ine ? Palibe wa imwe wamene anamiuza ngati mwana wanga wapanga chipangano na mwana wa Jessi. Palibe mwa imwe wamene anivelela chifundo ine. Palibe mwa imwe womiiza kuti mwana wanga atumfya wanchito wanga Davide kuti ani ukile. Lelo abisama nakuyembekeza kuti anichite chipongwe ine." ⁹ Apo Doegi mu Endomayiti, wamene ali imilile pamozi na wanchito wa Sauli anayankha kuti, "Ninaona mwana wa Jessi abwela ku Nobu, kuli Ahimelechi mwana wa Ahitubu. ¹⁰ Anapempha kuli Yehova kuti amuthandize, ndipo anamupasa zofunikila na Lupanga ya Goliyade mu Philisitina." ¹¹ Ndipo mfumu anatuma winangu kuti ayitane wansembe Ahimelechi mwana wa Ahitubu na wonse wakunyumba kwa atate wake, wansembe wamene anali mu Nobu. Wonse wanabwela kuli mfumu. ¹² Sauli anati, "mvela manje mwana wa Ahitubu, "Anayankha nilipana, mbuye wanga." ¹³ Sauli anati kuli eve, "wakanzelani upandu kuwavula ine, iwe na muona wa Jessi, pakuti wamupasa buledi, na Lupanga, ndipo kuti wapemphera kwa Mulungu kuti amuthandize, pakuti aniukile ine, kubisama mwachisinsi mwamene achitila masiku ano?" ¹⁴ Apo Ahimelechi anayankha mfumu makunena kuti, "Ndani pakati pa wachinto wanu wonse ali okhulupilika monga Davide, ndani mpongozi wa mfumu nakuti amalamulila ma bodigadi, ndipo niwolemekezeka munyumba mwanu?" ¹⁵ Kushe nikuyamba lelo kuti napemphela kuli Mulungu kuti aninthadize? Nchapatali kuchokela kwa ine !osaleka mfumu inivalike chilichonse ine kapolo wanu kapena yonse nyumba ya atate wanga. Pakuti kapolo wanu saziwako chilichonse za iyi nkhanu yonse. ¹⁶ Mfumu inayankha "zoona iwe uzafa, Ahimeleki, iwe na wonse wa munyumba mwa batate wako," ¹⁷ Mfumu inati kuli malonda wamene anali imilile momuzunguluka, "Piliukani Rakupaya wansembe wa Yehova. Chifukwa kwanja kwao naweve kuli na Davide, ndipo chifukwa wanaziwa kuti wathawa, koma sanaulule ichi kuli ine koma wachinto wa Sauli siwana chose kwanja kwao kupaya wansembe wa Yehova. ¹⁸ Apo mfumu inati kuli Doegu, "piliuka nakupaya wansembe." Apo Doegu mu Edomiti anapiliuka nakuyamba kucita chipongwe ansemb, anapaya eyite-fayivi wanthu woyala nyula yamapemphelo yalineni ephodi ija siku. ¹⁹ Anapaya futi nalupanga Nobu, muuzinda wa ansemb, babili wonse amuna na wakazi na bana natucheche, na ng'ombe zake zonse, mandonke na nkhusa anapaya na lupanga. ²⁰ Koma m'mozi wa wana wamuna wa Ahimelechi mwana wa Ahitubu, zina yake Abiathara, amazwenga nakuthawila kukonkha Davide. ²¹ Abiathara anauza Davide kuti Sauli anapaya onse ansemb a Yehova. ²² Davide anati kuli Abiathara, "Ninaziwa pa siku ija, pamene Doegu mu Edomayiti anali kwamene, kuti vazoona azauza Sauli. Ndine nalengesa imfa iliyonse yamene yachitika mubanja mwa atate wako! ²³ Nkhala na ine ndipo osayopa, pakuti wamene asakila sakila moyo wako askile na wanga futi. Uzankhala pamozi na ine kulibe chokuyofya chili chonse ndipo osachita mantha."

Chapter 23

¹ Wanamuza Davide kuti, "Ona ma Philisiti wali kumenyana na Keilaha nakuba mumalo opepetelamo vamumunda vanga." ² Apo Davide anapemphela kuli Yehova kupempha thandizo nakumufunsa eve, "Ningayende nakuwayamba nkondo awa na Philisiti?" Yehova anati kuli Davide, "yenda, nakuwayamba nkondo na Philisiti upulumunse Keilaha" ³ Wanthu wa Davide anati kuli eve, "Onani tiyopa kuno Yuda. Manje tikayenda ku Keilaha kuyambana na masoja wama Philisiti?" ⁴ Ndipo Davide anapemphela kuli Yehova kufuna thandizo na futi, Yehova anamuyankha "Nyamuka yenda ku Keilaha pakuti ine nizakupasa kugonjesa ma Philisiti." ⁵ Davide na wanthu wake anayenda ku Keilaha ndipo anamenyana na ma Philisiti, anapesela kutali ng'ombe zawo nakuwa kwapula na imfa ikulu maningi. Mwa ichi Davide ana pulumusa wanthu wonkhala mu Keilaha. ⁶ Pamene Abiathara mwana wa Ahimeleki anathawila kuli Davide ku Keilaha, anabwela na Ephodi mu manja mwake. ⁷ Sauli anauziwa kuti Davide anayenda ku Keilaha, Sauli anati, "Mulungu amupeleka mu manja mwanga. Pakuti niwovaliliwa ndawa angena mumuzinda wamene uli na ma geti kuyikililapo na mipilingisho." ⁸ Sauli ana sonkhanisa asilikhali kuti ayende kunkhondo, kuti ayende ku Keilaha, kuti akamuzunguluke mobisamila Davide na banthu wake. ⁹ Davide anaziwa kuti Sauli anali kukonzekela chiwembu pali eve. Anati kuli Abinthara wansembe, "Niletele ephodi kuno." ¹⁰ Niipo Davide anati, Yehova Mulungu wa Israeli, kapolo wanu namvela zooni kuti Sauli afuna kubwela ku Keilaha, kuti aworonge muzinda chifukwa cha ine. ¹¹ Kodi anthu aku Keilaha wazanipeleka ine mu manja mwake? Kodi Sauliazabwela kuno, monga mwamene kapolo wanu amvelela? Yehova, Mulungu wa Israeli, nikupapatani, chonde niuzeni nekapolo wanu." Yehova anati, "Azabwela kuno." ¹² Ndipo Davide anat, "Kushe wanthu waku Keilaha wazanisalenda ine na wanthu wanga mumanja mwa Sauli?" Yehova anati, "wazakupoleka iwe." ¹³ Apo Davide na banthu, wamene wanali pafupi chiwelengelo cha sikisi handedi, wananyamuka nakuchokamo mu Keilaha, ndipo wanayenda yenda kuchokela apa na apa. Chinauziwa kuli Sauli kuti Davide anali atathawa kuchoka ku Keilaha, ndipo awalekeza kumupitikisa. ¹⁴ Davide anali kunkhala mungaka za musanga, kumalo yakumalupili musanga yaku Ziphi. Sauli anali kumusakila siku, koma Mulungu sanamupeleke mumanja mwake. ¹⁵ Davide anaona kuti Sauli anatulikila kusakila umoyo wake; apo Davide anali musanga ya Ziphi pa Horesh. ¹⁶ Manje Jonathani, mwana wa Sauli, ananyamuka nakuyenda kuli Davide pa Horesh, nakulimbisa kwanja yako mwa Mulungu. ¹⁷ Anati kuli eve, "Osayopa, pakuti kwanja kwa Sauli tate wanga sikuzakupeza iwe. Iwe uzankhala mfumu yolamulila Israeli, ndipo ine nizankhala wachibili kuli iwe. Sauli tate wanga nayeve aziw futi za ichi." ¹⁸ Wanapanga chipangano pamenso pa Yehova. Davide anasala pa Hereshi, koma Jonathani anayenda kunyumba. ¹⁹ Maziphayiti anabwela kuli Sauli ku Gibeya nakunena kuti, "Kushe Davide sanabisame pakati pa ise kungaka zake pa Hereshi, pa lupili lwa Hakilaha, yamene ili ku m'mwala kwa Jeshimoni?" ²⁰ Apa bwelani mfumu! kulingana na chilaka chanu, bwelani kuno! Gawo yasu izankhala yomupeleka mumanja mwa a mfumu. ²¹ Sauli anati, "Mudalisike na Yehova ndawa manichitila chifundo ine." ²² Yendani, munkhale na chisimikizo chenicheni. Muziwe ndipo mufufuze kuti malo yake yo bisamapo yalikutu ndipo kuti ndani anamuona kwamene uko. Ninauziwa kuti niwochenjela maningi. ²³ Kansi kayang'anani nakuziwa zamayilo yonse kwamene amazibisa. Mukabwelele kuli ine na umboni weni weni, ndipo ine nizabwelela pamozi na imwe. Ngati alimo mu malo nizamusakila nakumutulusa kuchoka pa kati pa masauzande yonse ya Yuda." ²⁴ Ndipo wananyamuka nakuyenda pasogolo pa Sauli ku Zipha. Apa Davide na banthu wake anali musanga ya Maoni, mu Arabaha kum'mwela wa Jeshimoni. ²⁵ Sauli na wanthu wake wanayenda kumusakila. Koma Davide anauziwa za ichi, apo ana polikila kulupili yavimyala nakunkhala mu sanga yaku Maoni. Pamene Sauli anamvela za ichi anapikisa Davide mu Sanga ya Maoni. ²⁶ Sauli anayenda kumbali inangu ya lupili, ndipo Davide na wanthu wake wanchi kuyenda kudela inangu ya lupili ija. Davide anafulumila kuthawa kuchoka kunali Sauli. Pamene Sauli na banthu wake wanazunguluka Davide na banthu bake kuti awatenga, ²⁷ Mthenga anabwela kuli Sauli nakunena kuti, "fulumilani nakubwela, pakuti ma Philisiti wachita chipongwe choyamba nkondo mu ziko." ²⁸ Nchifukwa chake Sauli anabwelela kupitikisa Davide nakuyenda kumenyana nama Philisitina. Nchifukwa chake yaja malo yanayitaniwa kuti chi Mwala chozwengelako. ²⁹ Davide anakwezeka kuchokela uko nokunkhala mu ngaka zaku Enigedi.

Chapter 24

¹ Pamene Sauli anabwelela kuchoka kuputikisa ma Philisitina, anauziwa kuti "Davide ali mu sanga yaku Enigedi"

² Ndipo Sauli anatenga wanthu wali thiri sauzande amuna osankhindwa kuchokela kuli Israeli yonse,nakuyenda kusakila Davide na banthu wake ku myala ya Mbuzi zamusanga. ³ Anabwela kunakhola yankhosa munjila, pamene panali khevu. Sauli anangena mukati kuti avirunkhile mendo yake. Apa Davide na banthu wake anali nkhole kothela kwa khevu. ⁴ Banthu wa Davide anati kuli eve, "Lyi ndiye siku yamene Mulungu anakambapo pamene anati kuli iwe, 'Nizapeleka badani bako mu manja yako, pakuti iwe uchite naye mwamene ufunila.'" Apo Davide ananyamuka nakukalaba mwakachetechete kuyenda pasogolo nakujuwa kona ya mukhanjo wa Sauli. ⁵ Pasogolo pake Davide anavela mitima kuwawa chifukwa anajuwa nsonga ya mukhanjo wa Sauli. ⁶ Anati kuli banthu bake," Mulungu asachilole kuti ningachite ichi chinthu kuli mbuye wanga,wozozedwa wa Yehova, kutambulula kwanja yanga momuchita chipongwe,nitaona kuti niwozozedwa wa Mulungu. ⁷ Apo Davide anawazuzula wanthu wake na aya mau,ndipo sanawalole kumuyamba Sauli. Sauli ananyamuka,nakuchoka mu khevu,nakuyenda kwao. ⁸ Pasogolo pake Davide naye ananyamuka,nakuchoka mu khevu,nakuyitana mokuwa mbuyo mwa Sauli; "Ambuye wanga mfumu,"pamene Sauli anayang'ana kumbuyo kwake, Davide anawelama nankhope yake pansu nakuonesha ulemu. ⁹ Davide anati kuli Sauli, "Nchifukwa chani mumamvelela wanthu wamene wakamba kuti, 'Onani, Davide afuna kukuchitani choyipa?" ¹⁰ Lelo menso yanu yawona mwamene Yehova enze akuyikani mumanja mwanga,pamene tinali mu khevu. Wenangu wenze waniyuza kuti nikupayeni,koma wakulekelelani imwe,nakamba kuti,sini zatambasule kwanja yanga mochita chipongwe ambuye wanga, pakuti mwozozedwa wa Mulungu. ¹¹ Onani,atate wanga,onani nsonga ya mukhanjo wanu mumanja mwanga. Pa chifukwa chazooka kuti najuwako nsonga ya mukhanjo wanu nakusakupayani,imwe mungaziwe nakuona kuti kulibe choyipa kapena mulandu wowukila usogoleli mumanja mwanga,ndipo sininakuchimumwileni,ngaukhale kuti imwe muzengela moyo wanga kuti munipaye. ¹² Mulungu aweluze pakati pa imwe na ine,ndipo Mulungu azanibwezelamo kuli imwe m'malo mwanga,koma kwanja yanga sizakuchitani chipongwe imwe. ¹³ Monga mwambi wa wakudala ukamba kuti,'kunja kwa oyipa kumatuluka choyipa koma kwanja yanga siyizasusana na imwe. ¹⁴ Nindani wamene mfumu ya Israeli ya chokela kunja? Mupitikisa ndani? Mukonkha galu wakufa? Mupitikisa inda? ¹⁵ Mulungu ankhale woweluzo ndipo apase chiweluzo pakati kaimwe na ine,nakuona kuti anikambilako zofuna zanga,na kunilola kuti nizwenge kuthawa kwanja yanu." ¹⁶ Pamene Davide anasiliza kukamba aya mau kuli Sauli , Sauli anati , " Nimau yako ayo , mwana wanga Davide ?" Sauli anakweza mau yake nakulila. ¹⁷ Anati kuli Davide , "Niwe olungama maningi kuchilapo ine , pakuti wanilipila chabwino ine , pamene ine ninakulipila choyipa. ¹⁸ Waulula lelo mwamene wachitila zabwino kwa ine , pakuti sinunanipaye pamene Yehova enze aniyika mu chifundo chako. ¹⁹ Pakuti ngati munthu apeza mudani wake angamusiyiye kuti ayende mumtendele ? Mulungu akulipile chabwino pa chamene wachita kwa ine lelo. ²⁰ Apa , ine naziwa kuti iwe uzankhala zooka mfumu nakuti ufumu wa Israeli uzankhauzankhazikisiwa mumanja mwako. ²¹ Ulapile kwa ine kuti siuza juwa kusilizilatu mbadwo wanga wamene ukonkha ine nakuti siuza ononga zina yanga kuichosa pa banja ya batate wanga." ²² Apo Davide analapa njazi kuli Sauli . Ndipo Sauli anayenda kwawo, koma Davide na wanthu wake anayenda kungaka yawo.

Chapter 25

¹ Manje Samueli anafa . Israeli yonse inalongana pamozi nakulila malilo ya Samueli , ndipo wanamushika panyumba pake ku Rama . Apo Davide ananyamuka nakuyenda ku sanga ya Parani. ² Kunali mwamuna ku Maoni , wamene katundu wake wenze ngomila . Uyu munthu anali thiri sauzande na mbuzi zili wanu sauzande . Anali kuwetela nkhusa zake ku Camelo. ³ Zina ya uja munthu inali Nabala , ndipo zina ya mkazi wake inali Abigailo. Uyu mkazi anali wanzelu maningi ndiponso wakongola m'maonekedwe ake . Koma mwamuna wake anali wankhanza ndiponso wa maganizo oipa muzichitidwe zake . Anali mbadwa yakunyumba ya Caleb. ⁴ Davide anamvela munsanga mwamene analili kuti Nabala anali kuwetela nkhusa zake. ⁵ Apo Davide anatuma anyamata wake wali teni . Davide anati kuli anyamata , "Yendani ku Camelo , yendani kuli Nabala , nakumu pasa moni muzina yanga . ⁶ Muzakamba kuli eve kuti , " Uzinkhala mu chitukuko , mtendele kwa iwe nakuli amunyumba mwako , ndipo mtendele pali vonse vamene uli navo. ⁷ Nimvela kuti na achiweta , achiweta wanu anali na ise , ndipo sitinawachite choyipa , ndipo palibe chamene chinasowapo panthawi yonse yamene wanali ku Camelo. ⁸ Funsani anyamata wanu , ndipo azakuuzani . Lomba lekani anyamata wanga wepaze chikondi m'meso mwako , pakuti tafikapa siku yachisangalalo. Chonde tipasani koni vili vonse vamene muli navo m'manja mwanu kuli akapolo wanu na kuli mwana wanu mwamuna Davide. " ⁹ Pamene anyamata wa Davide anafika , wanakamba zonse izi kuli Nabala m'malo mwa Davide nakuyembekeza. ¹⁰ Nabala anayankha anyamata wa Davide , "Davide nindani , ndipo mwana wa Jessi nindani? Kuli akapolo wambili m'masiku wano wamene wazichosa kuli a mbuye wao. ¹¹ Kuse ine ningatenge buledi yanga , na manzi yanga , nanyama yanga yamene napayila achiweta wanga , nakuyipeleka kuli wanthu wamene siniziwa kwamene wanachokela ?" ¹² Apo anyamata wa Davide wanabwelela naku yenda kumuza zonse zamene zina kambika . ¹³ Davide anati kuli anyamata wake , " Munthu aliyense amangilile lupanga yake , " ndipo munthu aliyonse anamangilila lipanga yake . Pafupi folo hundredi amuna wanakonkha mu mambuyo mwa Davide . Koma twu hundredi wana salila makatundu. ¹⁴ Koma m'mozi wa anyamata anauza Abigailo , mkazi wa Nabala ; anati , " Davide anatuma anthenga kuchoka kusanga kubwela mkuposha bossi wathu , koma weve awanyoza. ¹⁵ Koma awa wanthu wanali nachifundo maningi kuli ise . Sanatichite choyipa ndipo sipanasowe chilichonse malingana tinali kuyenda nawo pamene tinali musanga. ¹⁶ Anali chiwumba chathu pawili ponse muzuwa na usiku , nthawi yonse yamene tinali nawo kusamalila nkhusa. ¹⁷ Nchifukwa chake muchiziwe ici nakuganizila vamene muzachita , ndawa choyipa chikonzekelewa a bossi wathu , ndiponso choyipa chizachitikila nyumba yawo yonse . Nimunthu u wachabe chabe alibe ulemelelo uliwonse kwakuti kulibe munthu anga mwelane naye. " ¹⁸ Apo Abigailo ana fumila nakutenga mikate ili twu handredi , mabotolo awili ya wayini , mbelele zili fayivi zo fundula kudala , mipimo fayivi ya chimphonde , tumeda wanu handredi twa masuku yoyanika , na twu handredi tumakeke twa nkhuu , nakuvikwezeka pa donke. ¹⁹ Anati kuli anyamata wake , "Tiyeni pasogolo panga , ndipo nizamukonkhani mumambuyo mwanu . " Koma sanauze mwamuna wake Nabala. ²⁰ Pamene anali kuyenda okwela pa donke anatelemukila pa mitengo yophimba lupili , Davide na wanthu wake ana seluka kulungama kwamene analili , ndipo anakumana nawo. ²¹ Apo Davide enze anakamba kuti , " Nzoona kuti ninalikulonda vonse vamene uyu munthu ali navo papanda phindu musanga , pakuti kulibe chinasowapo pavonse vamene vili vake uyu munthu , koma anibwezela choipa m;malo mwa chabwino. ²² Mulungu achite telo kuli ine , Davide ndipo maningi achite choncho , ngati po fika kuseni nizasiyako loko mwamuna akwana umozi mwa wonse wanthu wake." ²³ Pamene Abigailo anaona Davide , anafulumila nakuseluka pa donke na kugona choyang'ana nkhope pansi ndipo nakuziwelamisa yeka pansi. ²⁴ Anagona pamapazi yake nakunewa kuti , "Pali ine chabe , ambuye wanga , ndiye pazankhala mulandu. Chonde ndipo mvelani kumau ya kapolo wanu. ²⁵ Musalole mbuye wanga kuganizila ichi chipuwa chilibe nchito , Nabala , pakuti ndiye chamene zina yake ikamba , ndiye vamene alili . Nabala ndiye zina yake , ndipo upuba ulinayeve . Koma ine kapolo wanu siniwaone anyamata wa ambuye wanga wamenemwenze mwatuma . ²⁶ Apa manje , a mbuye wanga , malinga Mulungu niwamoyo , ndipo na imwe pamene muli na moyo , pakuti Mulungu akulesani kukhesa mwazi , na kuti musabwezemo mweka mumanja yanu , apa lekani adani wanu nawaja wamene wasakila kuchita choipa kuli mbuye wanga , ankhale monga Nabala. ²⁷ Manje lekani iyi mphaso yamene kapolo wanu aleta kuli mbuye wanga ipasiwe kuli anyamata wamene wakonkha ambuye wanga. ²⁸ Napapata khulunkani zolakwa zakapolo wanu , pakuti Yehova azapanga loko chinkhale bwanji ambuye wanga kunkhala nyumba ya zooni , chifukwa ambuye wanga muli kumenya nkondo za Yehova ; ndipo choyipa sichizapezeka muli imwe malingana ndimwe wamoyo. ²⁹ Angankhale wanthu wanyamuka kukupitikisani imwe kuti akupangeni , koma moyo wa mbuye wanga uzamangililiwa mumtolo wa amoyo na Yehova Mulungu wanu ; nndipo azavulumulila kutali myoyo ya adani wanu , monga kuchokela muchikwama cha chovulumula. ³⁰ Yehova azakachitila a mbuye wanga zonse zamene anakulonjezani imwe , ndipo akusonthani imwe kunkhala musogoleli

wa Israeli. ³¹ Ichi sichizankhala chisendo cho zezeleka nacho kuli imwe - kuti mwakhesa pansi mwazi wakaye , kapena chifukwa mbuye wanga munayeselela kuzi pulumusa mweka . Pakuti pamene Yehova azachita chabwino kuli mbuye wanga , mukakumbukile kapolo wanu. " ³² Davide anati kuli Abigailo, " Adalisike , Yehova , Mulungu wa Israeli , yeve wamene wakutuma kuti ubwele kukumana naine lelo. ³³ Nzelu zako nizodalisika na iwe niwe odalisika , chifukwa wanileselela mkuyenda kukhesa mwazi nakuyenda kubwezamo neka nakwanja kwanga kuli adani wanga. ³⁴ Pakuti mwa choonashi , Malingana Yehova , Mulungu wa Israeli , mwamoyo , yeve wamene wanilesa ine kuti nisakuchite choyipa mpaka wachita changu kubwela kukumana na ine , sembe zoona sikunasalepo kwa Nabala nangu babyi m'mozi mwamuna poyenda kufika kuseni. " ³⁵ Apo Davide analandila kuchoka mkwanja kwake chamene anabwelesa kuli eve : anati kuli eve , "Yenda ukwezeke mumtendele kunyumba kwako ; ona ine namvela mau yako mau yako ndipo nakuvomela iwe. " ³⁶ Abigailo anabwelela kuli Nabala ; onani , anali kuchita phwando munyumba mwake , monga pwando yamfumu ; ndipo mtima wa Nabala unali wokondwa mkati mwake , pakuti anakolewa maningi , apo sanamuuze kalikonse mpaka kwacha kuseni. ³⁷ Chinabwela kuchitika kuseni , pamene wayininali itamuchoka Nabala, kuti mkazi wake anamuwuza izi zinthu ; mutima wake unafa mkati mwake , ndipo anasanduka monga mwala. ³⁸ Chinabwela kuchitika panapita masiku pafupi teni pasogolo pake kuti Yehova anamuchita chipongwe Nabala ndipo anafa. ³⁹ Pamene Davide anamvela kuti Nabala anamwalila , anati , "Yehova alemekezeke, wamene achitapo kanthu pa manyozo yanga kuchokela mu zanja ya Nabala nakusunga kapolowake kuti asachite choyipa . Atembenula choyipa chinachita Nabala kumubwezela pamutu pake." Apo Davide anatuma nakukamba na Abigailo , kuti amutenge kuli eve ankhale mkazi wake. ⁴⁰ Pamene wanchito wa Davide anabwela kuli Abigailo pa Carmelo , wanakamba naye na kunena kuti, "Davide atituma kuli iwe kuti tikutenge kuli eve ukamkhale mkazi wake." ⁴¹ Ananyamuka , nakuwelama eve mwine nachinso chake pansi , na kunena kuti, "Onani kapolo wanu mukazi nikapolo wosauka ma pazi wa wanchito wa a mbuye wanga." ⁴² Abigailo anafulumila kunyamuka , nakukwela pa Donke na wanchito wake wakazi wali fayivi wamene wanamukonkha ; ndipo anakonkha anthumwi wa Davide , ndipo anankhala mkazi wake. ⁴³ Apo Davide anali atatenga futi Ahinoamu waku Jezreeli kunkhala wazikazi wake . ⁴⁴ Naye Sauli anali atamupeleka Michala mwana wake , mkazi wa Davide kuli Palatiele mwana wa Laishi , wamene anali waku Gaulimu.

Chapter 26

¹ Maziphiti anabwela kuli Sauli pa Gibeya na kunena kuti, " Kushe Davide sali wobisama mulupili lwa Hakila , yamene ili tikalibe kufika ku Jeshimoni?" ² Apo Sauli ananyamuka nakuyenda kupolikilala kusanga yaku Ziphi , ali na thri sauzande wanthu wesankhindwa wamu Israeli pamozi naye , kufuna Davide mu sanga ya Ziphi. ³ Sauli anamanga misasa pa lupili lwa Hakila , yamene ili mukalibe kufika ku Jeshimoni , pambali pa musewu . Koma Davide anali kunkhala mu sanga , ndipo ana ona kuti Sauli anali kubwela kukonkha eve musanga. ⁴ Apo Davide anatuma akamuchoke nakuziwa kuti Sauli wabwela zoona . ⁵ Davide ananyamuka nakuyenda kumalo kwamene Sauli anali atakhoma misasa; anaona pamalo pamene Sauli anagona ,na Abinala mwana wa Neli, Genero wa Gulu yake yankhondo ; Sauli anagona mu musasa , ndipo wanthu wana khoma misasa mumuzunguluka , wonse wogona. ⁶ Apo Davide anati kuli Ahimelechi mu Hihiti , na kuli Abishai mwana wa Zerua , mbale wa Joab , " Ndani aza seluka na ine kuyenda kuli Sauli mumusasa ?" Abishai anati , "Ine ! Ine nizaseluka na imwe. ⁷ Apo Davide na Abishai anayenda kuli masoja usiku , Sauli analiko atagona mu m'kati mwamisasa namkondo wake wolasa pansi pa fupi na mutu wake . Abinala na masoja wanangu momuzunguluka . ⁸ Apo Abishai anati kuli Davide , " Lelo Mulungu ayika mudani wake mumanja yako . Apa chonde lekani nimuphinile pansi na mukondo nankhonya imozi chabe . Sinizamuchaya kachiwili." ⁹ Davide anati kuli Abishai , " Osamuononga pakuti nindani angatambasule kwanja yake kuchitila chipongwe ozozedwa wa Yehova nakunkhala alibe mulandu? " ¹⁰ Davide anati , "Malingana Yehova niwamoyo , Mulungu azamupaya yeka ,kapena siku yake izafika yokufa , kapena azayenda ku nkondo nakufa kwamene uko. ¹¹ Mulungu asachilole kuti ine nitambasule kwanja kwanga mosusana na wozozedwa wake ; koma apa , nikupempha iwe , tenga mukondo wamene uli kumutu kwake na chikapu chamanzi , ndipo tiyeni tiyende. ¹² Apo Davide anatenga mkondo na chikapu cha manzi kuchosa kumutu kwa Sauli , ndipo wanachokapo . Kunalibe futi aliyense wamene anauka , pakuti wonse wanali mtulo, chifukwa tulo kwakuya tochokela kuli Mulungu twenze tunawagwela weve. ¹³ Choncho Davide anayenda kumbali inangu yalupili na kuyimilila pa mwamba patali ; panali chimutunda chikulu pakati pawo. ¹⁴ Davide anapunda kuli banthu na kuli Abinala mwana wa Neri ; anati , " Siuyankha , Abinala ?" Apo Abinala anayankha kunena kuti , " Ndiwe ndani nindani wamene akuwa kuli mfumu?" ¹⁵ Davide anati kuli Abinala , " Sindiwe munthu alibe mantha ? Ndani wamene ali monga iwe mu Israeli ? Ndani ndipo kuti siunamuyang'anile mbuye wako mfumu? pakuti winangu enze abwela kuti apaye mfumu a mbuye wako. ¹⁶ Ichi chinthu chamene wachita sichabwino . Malingana Yehova niwamoyo iwe ufunika kufa chifukwa sinakwanilise kulonda a mbuye wako , wozozedwa wa Yehova . Manje ona kwamene kuli mkondo wa ambuye wako na chikapu cha manzi vamene venze kufupi namutu wako!" ¹⁷ Sauli anaiziwa liwu ya Davide nakunena kuti , " Aya nimau yako , mwana wanga Davide ?" Davide anati , " Nilizu yanga , ambuye wanga , mfumu ." ¹⁸ Anati , " Nchifukwa chani ambuye wanga mupilikisa kapolo wanu ? Nachita chani ? Muli chimo yanji mumanja mwanga ? ¹⁹ Nchifukwa chake apa manje nipempha kuli imwe , lekani ambuye wanga a mfumu amvelelele kuli mau ya kapolo wanu , ngati ni Yehova wamene akuvundwani imwe pali ine kuti munichite chipongwe ine , lekani avomele chopeleka ; koma ngati nimunthu atembeledwe mumensomwa Yehova, pakuti lelo wanipitikisa kunja , kuti ine nisagwililile ku chokolo chakwa Yehova ; wakamba kuti kuli ine , 'Yenda ukapembeze milungu inangu.' ²⁰ Kansi manje nchifukwa chake , osaleka mwazi wanga ugwele pansi kutali na chinso cha Yehova ; pakuti mfumu yaku Israeli yabwela kunja kusakila nsanya imozi monga mwamene wina azangelela nkwale yamumalupili." ²¹ Apo Sauli anati , " Nachiwa , bwelela , Davide mwana wanga ,pakuti sinizakuchita futi choyipa , chifukwa moyo wanga waoneka wamtengo wapatali m'menso mwako lelo . Ona , na sobela uchipuba na kupanga misiteki yoyipa maningi." ²² Davide anayankha nakukamba kuti , " Onani mkondo wanu ulikuno , mfumu ! Lekani m'mozi mwa anyamata abwele kuno na kuwutenga akuleteleni kwamene mulili. ²³ Mulungu amupase munthu aliyonse pali chilungamo chake nakukhulupilik kwake ; chifukwa Yehova enze akuyika mumanja mwanga lelo , koma sininapaye wozozedwa wake. ²⁴ Onani , mwamene umoyo wanu wenze wa mutengo wapatalimumenso mwanga lelo , ndiye mwamene umoyo wanga uneke wa phindu maningi m 'menso mwa Yehova ,ndipo anipulumuseko ine kunichosa mu mavuto yonse ." ²⁵ Apo Sauli anati kuli Davide , "Udalisike , Davide mwana wanga ! Uzachita zoona vikulu ndipo uzakwanilisa mkunichita ." Apo Davide anayenda njila yake , ndipo Sauli anabwelela kwao.

Chapter 27

¹ Davide anatii m'mtima mwake , " Ine manje nizafa siku inangu nakwanja kwa Sauli ; palibe chabwino chili chonse kuli ine kupalapo kuti ine nizwengele mu malo ya ma Philisiti ; Sauli azasalenda kunisakila futi mkati mwa malile ya Israeli njila iyi nizathawa kuchoka mumanja mwake. ² Davide ananyamuka naku pitilila , eve na wanthu sikisi handredi wamene wanali naye , kuli Achishi mwana wa Maoki , mfumu yaku Gath. ³ Davide anali kunkhala na Achishi pa Gath , eve na banthu wake , mwamuna aliyonse na wamunyumba mwake , ndipo Davide na aszikazi wake wabili , Ahinoam muzimayi waku Jezreeli, na Abigailo muzimayi waku Carmelo , wamene anali mkazi wa Nabala. ⁴ Sauli anauziwa kuti Davide anathawila ku Gath , nchifukwa chake sanali kumusakila nafuti manje. ⁵ Davide anati kuli Achishi , " Ngati napeza chifundo m'menso mwanu , nipasanikoni malo mu imozi mwa mizinda chamusanga , pakuti nizinkhala pamene apo. Nchifukwa chanji ine kapolo wanu nizinkhala mumuzinda wachifumu pamozi na imwe? " ⁶ Ndiye iyo siku Achishi , anamupasa zikilagi ; nichifukwa chake zikilagi niyawo mafumu yaku Juda mpaka lelo. ⁷ Nambala ya masiku yamene Davide anankhala mu ziko ya ma Philistina inali chaka chimozi na myezi folo. ⁸ Davide na wanthu wake wanali kuchita nkondo mumalo osiyana siyana , kuchita chipongwe ma Geshurayiti, ma Girizayiti, ma Amalekayiti; pakuti iyo mitundu ndiye inalikunkhala mumalo pamene muyenda chaku Shuri , mpaka ku ziko yaku Egypiti . Wanalikunkhalamo umu mumalo kuchokela kale. ⁹ Davide anayenda kuchita nkondo na ija ziko ndipo sanasiyepo mwamuna loko mukazi wamoyo. Anatenga nkhoa , nang'ombe , madonke , na zovala kuyenda navo . Ndipo eve anabwelela nakuyenda kumbuyo kuli Achishi. ¹⁰ Achishi anakonda kukamba kuti , " Nindani wamene wayenda kuchita nkondo lelo?" Davide anali kuyankha , " Namenyana na kumwela kwa Juda , " kapena "namenyanana na kumwela kwa Jerahmeelayiti , " kapena "namenyanana na kumwela kwa ma kenayiti." ¹¹ Davide sanali kusiyako mwamuna kapena mkazi kuti awabwelese ku Gath , kunena kuti , " Pakuti siwangakambe pali ise kuti,' Davide anachita chaso na chaso.'" Ichi nichamene anachita nthawi yonse yamene anali kunkhala muziko yama Philisiti. ¹² Achishi anakhulupilila Davide kunena kuti , " Alengesa wanthu wake waku Israeli kunyansiwilitu naye; nichifukwa chake azankhala kapolo wanga kwamuyaya."

Chapter 28

¹ Chinabwela kuchitika masiku amene ayo kuti A Philisiti anasonkhana masoja wawo pamozi kuti achite nkondo kumenyana na Israeli. Achishi anati kuli Davide , "Uchiziwe ichi mopanda chikayiko kuti uzayenda na iwe mugulu ya bankhondo , iwe na masoja wako." ² Davide anati kuli Achishi , " Ngati niso , muzaziwa chamene kapolo wanu angachite ." Achishi anti kuli Davide , "Nishi ine nizakupanga bodigadi wanga masiku yako yonse yaumoyo." ³ Apa Samueli anali atamwalila , ndipo Israeli yonse inamulila eve nakumuika mumanda yaku Rama , mumuzinda wakwao. Naye Sauli , anali atapitikisa kuwachosa muziko wonse wanthu wamene wanali kukamba nawakufa kapena kukamba na mizimu. ⁴ Apo a Philisiti anazikolonganika pamozi nakubwela ndipo anankhoma misasa yawo pa Shunemu ; ndipo Sauli anasonkhanisa Israeli yonse pamozi , ndipo anamanga misasa pa Gilubowa ⁵ Pamene Sauli anaona gulu ya wankhondo yama Philisiti , anachita mantha , ndipo mutima wake unanjenjemela maningi. ⁶ Sauli anapemphela kwa Yehova kufuna thandizo, koma Mulungu sanamuyankhe - osati kupitila mumaloto kapena mu chimubuluso kapena aneneli. ⁷ Apo Sauli anati kuli atumiki wake , " Nipezelenikoni muzimayi wa mizimu , pakuti ningayende kuli eve nakufunsa malangizo wake ." Atumiki wake anati kuli eve , "Onani aliko mukazi wa ku Endo wamene na zimvela kuti anakambisana na wakufa." ⁸ Nchifukwa chake Sauli anazibisa , pakuvala vovala vachabe chabe nakuyenda , eve na wamuna awili anali naye . Anayenda kuli uja mukazi usiku. Anati , " Niwombezeleko namuzimu ndipo uniwukisileko kuchokela kuli wakufa wamene nizatoma." ⁹ Uja mukazi anati kuli eve , " Ona , uziwa zamene Sauli anachita , mwamene analesela nakupitikisila kuchokela muziko waja wamene wakamba na wokufa na mizimu . Manje nichani uteya musampha pa moyo wanga , kuti unipayise?" ¹⁰ Sauli analapila kuli eve mzina ya Yehova nakunena kuti , "Malingana Yehova niwamoyo , kulibe chilangiso chizakuchitikila iwe kamba ka ichi chinthu." ¹¹ Apo muzimayi anati , " Nikuwushila ndani kuchokela kwa akufa ?" Sauli anati , "Niushileko Samueli ine." ¹² Pamene muzimu anaona Samueli , anapunda na mau yokwela nakukamba na Sauli, kuti , " Waninamizila chani ? Pakuti ndiwe Sauli." ¹³ Mfumu anati kuli eve," Osayopa . Waona chani? " Muzimayi anati kuli Sauli , "Niona mulungu achoka kunja kuchokela mudothi." ¹⁴ Anati kuli eve , " aoneka bwanji ? " Eve anayankha kuti , " Mwamuna wakalamba afukuluka ; niwovalikiwa mukhanjo ." Sauli anaziwa kuti anali ni Samueli , ndipo anawelama nkhope yake kuchita kufika pansi , nakumuonesha ulemu. ¹⁵ Samueli anati kuli Sauli , " Wanisokoneza na kuniwushila chani? " Sauli anayankha , " Nine wotekeseka maningi , pakuti a Philisiti akonzekela kuchita nkondo naine , ndipo Mulungu anithawa nakuti aleka kuniyankha vilivonse , kosati kupitila muli aneneli , nangu kupitila mumaloto . Nchifukwa chake nakuyitanani imwe ,kuti munganiziwise ine vamene nizachita." ¹⁶ Samueli anati , "Nanga ine nishi unipempha chani pakuti Yehova akuthawa nakusanduka ndani wako? ¹⁷ Yehova achita kwa iwe chamene anakamba kuti azakachita . Yehova ang'ambaku ufumu kuchosa mukwanja kwako nakupasa weve kuli munthu winangu - kuli Davide. ¹⁸ Chifukwa iwe suuna mvelelele mau ya Mulungu nakuti siunachite mkwiyo wake woyofya ma Ameleki , nchifukwa chake achita ichi kuli iwe lelo. ¹⁹ Yehova azapeleka Israeli pamozi na iwe mumanja yama Philisiti , ndipo mailo iwe na bana wako wamuna muzayamba kunkhala na ine kuno.Yehova azapeleka nayeve gulu ya masoja ya Israeli mumanja mwa ma Philisiti." ²⁰ Ndipo Sauli pamene apo anagwa nyutu pansi ndipo anakomoka chifukwa cha mau a Samueli . Anasila mphamvu chifukwa sanadye kanthu ija siku , angankhale uja usiku wonse. ²¹ Uja muzimayi anabwela kuli Sauli nakuona kuti anali wovutika maningi , anati kuli eve , "Ona , kapolo wako mukazi akumvela mau yako; naika moyo wanga mukwanja kwanga ndipo namvela mau yako yamene wakamba kuli ine . ²² Manje nichifukwa chake , niku papata iwe , naiwe mvelelele mau yakapolo wako mukazi , ndipo leka nikupase tuchakudya tung'ono pali iwe . Udye pakuti unkhale namphamvu pakuti ukayende njila yakwanu." ²³ Koma Sauli anakana nakunena kuti , " Sinizadya ." Koma wanchito wake pamozi na uja muzimayi ,wamamufosing'a , ndipo anamvela kuli mau yao. Apo anauka kuchokela pansi nakunkhala pa bedi. ²⁴ Muzimayi anali na kang'ombe koyina panyumba ; anafulumila nakukapaya ; anatenga unga wa tilingu , nakuwukanya tuma bola , nakupanga buledi ilibe chotumphisila muli tumabola twamene . ²⁵ Analeta vija vakudya pali Sauli na wanchito wake , ndipo wanadya . Ndipo wananyamuka na kuyambapo wamene uja usiku.

Chapter 29

¹ Apo ma Philisiti anakolonganika maasoja wao wonse pa Apheki, ndipo Israeli anamanga misasa pafupi na nyenja zamanzi zamene zili pa Jezreelu. ² Akazembe wama Philisiti anapitila pafupi na ma hundredi nama sauzande; Davide na wanthu wanapita kunkonkha mumbuyo mwa gulu yoteteza Achishi mumambuyo. ³ Ndipo akazembe wama Philisiti anati, "Awa ma Heberi acita chani kuno?" Achishi anati kuli akazembe wanangu wama Philisiti, "Kushe uyu si Davide, wanchito wa Sauli, mfumu ya Israeli, wamene ankhala na ine masiku onse awa, kapena kukwanisa na zaka, ndipo sininamupeze na cholakwa kuchokela pamene anabwela kwa ine mpaka siku yalelo?" ⁴ Koma asogoleli wama Philisiti anamukalipila maningi na kunena kuti, "Uyu munthu mubwezeni kumbuyo, pakuti abwelele kumalo yamene munamupasa. Sazayende naise kunkhondo, ndaba azatyalukila panthawi yomenyana. Nanga kuli njila yabwanji inangu yamene angazibwezele kuli ambuye wake koposa kuti akapeleke mitu yabanthu wathu pakuti amubvomele futi?" ⁵ Kushe uyu si Davidde wamene enzoyimbilana nyimbo weka weka povina kunena kuti, 'Sauli anapaya wake masauzande' ndipo Davide yake mateni sauzande?" ⁶ Apo Achishi anaitana Davide pambali na kumuza kuti, "Malingana Yehova niwamoyo, wenze wabwino kuli ine, ndipo kuchoka kunja kwako nakungena mkati kwako na ine mu gulu yamasoja nikwabwino mukuona kwanga pakuti sininapezepo cholakwa pali iwe kuchokela soki yakubwela kwako kuli ine mpaka pasiku yamene iyi yalelo. Loko kuti chili muli uyu musango, azisogoleli wa ma Philisiti sanakondwele naiwe." ⁷ Apa so bwelela nakuyenda mumtendele, pakuti usakhumudwise nduna zama Philisiti." ⁸ Davide anati kuli Achishi, "koma nalokwa cani? mwapezamo chani muli kapolowanu malingana pamene nenze naimwe kufika mpaka lelo, pakuti siningayende nakumenyana na badani wa mbuye wanga mfumu?" ⁹ Achishi anayankha nakunena kuli Davide, "Niziwa kuti ulibe cholakwika mkuona olo monga niwe ngelo wa Mulungu; koma olo nichoncho; akazembe wama Philisiti wakamba kuti, 'Asayende na ise kunkhondo.'" ¹⁰ Apa manje uwuke kuseni seni na wanchito wa a mbuye wako wamene wabwela na iwe; malingana ukauka kuseni seni m'mawa nakuti kuoneka, muyende." ¹¹ So Davide anauka m'mamawa, eve na masoja wake, kuyambapo m'mawa, kubwelela ku ziko ya ma Philisiti. Koma ma Philisitina wanakwezeka mpaka ku Jezireelu.

Chapter 30

¹ Chinachitika , pamene Davide na masoja wake wana bwelela ku Zikilagi pa siku yachitatu , ma Amaleki anali atathira nkondo kumalo ya Negevu na pali Zikilagi, anamenya Zikilagi nakuishoka, ² nakugwila mazimayi na aliyense wamene analimo , bonse babili wang'ono nawakulu . Sanapayepo aliyense , koma anawapesa wonse pamene anali kubwelela njila yakwao. ³ Pamene Davide na banthu wake wanabwela ku muzinda , inaliyoshokewa , ndipo azikazi wawo , na wana wao wamuna , na wana wawo wakazi wanali atatengedwa ukayili. ⁴ Apo Davide na wanthu wonse wanali eve anakweza mau yawo nakulila mpaka wanalibe futi mphamvu yolila. ⁵ Azikazi wawili wa Davide wanatengaewa ukayili , Ahinoamu mkazi waku Jezireelu na Abigailo mkazi waku Carmelo enze wa Nabala. ⁶ Davide anavutika maningi , pakuti wanthu wenze pangana zakuti wamuteme nyala , ndaba wonse wanthu wenze wekhumudwa mumuzimu , munthu aliyense pa bana wake wamuna na wakazi ; koma Davide anazilimbikisa eve yeka muli Yehova Mulungu wake. ⁷ Davide anati kuli Abithara mwana wa Ahimelechi , wansembe , " Nakupapata leta ephodi pano kuli ine." Abithara analeta ephodi kuli Davide . ⁸ Davide anapemphela kuli Yehova kufunsa zocita anati , " Ngati nizapitikisa iyi gulu ya ankhondo , nizawapeza? " Mulungu anamuyankha , " Pilikisa , pakuti uzawapitilila zoona , ndipo uzapuluma zonse palibe chikayiko." ⁹ Apo Davide anayenda , anali na masoja sikisi handredi pamozi na eve , anafika kukamana Besori, pamene waja wanasalila wanankhala . ¹⁰ Koma Davide anapitiliza kupitikisa , enze na banthu wali folo handredi ; chifukwa twu handredi wanasalila wenze wofoka maningi kwa kuti siwa natauke kamana ka Besori . ¹¹ Wanapeza mu Egipti musanga nakumubwelela kuli Davide ; anamupasa buledi ndipo anadya nakumupasa manzi yakumwa; ¹² ndipo anamupasa kadunswa ka keke ya nkhuu na tumipimo tubili twa viwaya . Atasiliza kudya , anankhala namphavu futi , pakuti sienze anadya buledi iliyonse kapena kumwa manzi kwa mzuwa mutatu na usiku utatu. ¹³ Davide anati kuli eve, " Kushe iwe ndiwe wa kuli ndani ? uchokela kuti? " Eve anayankha kuti , ndine m'nyamata waku Egipti , wanchito kuli mu Amaleki , bossi wanga ananisoya ine chifukwa masiku atatu aya yapita ninadwala. ¹⁴ Tinangenela nakupoka vinthu pa ija Negevu yama Kerethiti , navamene viliva ma Yuda , na Negevu ya Calebu , ndipo tinashoka Zikilagi." ¹⁵ Davide anati kuli eve , " Iwe unganisogolele kuli iyi gulu yankhondo ?" Mu Egipti anati , "Ulape kuli ine muzina ya Mulungu kuti siuzanipaya kapena kunigulisa ine mu manja mwa a bossi wanga , ninsi ine nizakupelekezani kuli aba wakabwalala." ¹⁶ Pamene mu Egipti analangiza Davide kufika vipondo venze vomwazikona pamalo ponse pnsi , kudya na kumwa nakuvina chifukwa cha vinthu vonse vumene wanapoka kuziko ya ma Philisiti na kuchokela kumalo ya Juda. ¹⁷ Davide anawamenya kuchokela mumazulo pa mungena kwa kazuba mpaka mumazulo mwa siku yokonkhapo . Kulibe munthu anathawa kupatulapo anyamata bali folo handredi , wamene wanakwela pali ma camelo nakuthawa. ¹⁸ Davide anapolola vonse vumene ma Amaleki wenze wanatenga ; nafuti Davide anapolola azikazi wake wawili. ¹⁹ Palibe chamene china shota , ching'ono loko chikulu , osati wana wamuna loko wakazi , osati viweto vopokewa pankhondo loko nangu chilichonse chamene wakawalala wenze wanazitengela wanewake . Davide anavibweza vonse. ²⁰ Davide anatenga gulu yonse yankhosa na gulu yonse yang'ombe , vumene wanthu wanapesela pasogolo pa viweto vinangu . Wanakamba kuti , " Ivi ni viweto votengewa pa nkondo va Davide ." ²¹ Davide anafika pali masoja yali twu handredi wamene wenze wofoka maningi kuti wamukonkhe waja wamene masoja wanzawo wanawasalisa pa kamana ka Besori . Awa wanthu wanayenda pasogolo kuti akumane na Davide na masoja wenzelili naye . Pamene na Davide anafika kuli aba wanthu , anawaposha. ²² Apo wonse wanthu woyipa mitima na waja banthu wachabe chabe pakati pa waja wamene wanayenda na Davide wanakamba kuti , " Chifukwa awa wanthu siwanayende na ise , sitizawapasako chilichonse chamene tapokoshola . Koma chabe , mwamuna aliyense atengepo akazi wake na wana wake nakuyenda." ²³ Apa Davide anakamba kuti , "Osachita so ; azibale wanga , na chamene Mulungu watipasa . Atisunga moyo ife nakutipasa mumanja mwatha wakawalala wamene wanabwela kuli ise mwachipongwe. ²⁴ Kulibe wamene azakubvomelezani muli iyi nkhani? Pakuti mwamene izankhalila gawo ya wamene enze kunkhondo chimozi gawo ya wamene wenze wankhala kulindila vimachola ; wonse wazagawana nakugawana molingana." ²⁵ Nimwamene chinankhalila kuchokela ija siku mpaka lelo , pakuti Davide anachipanga kunkhala lamulo na chonkhazikisidwa mu Israeli. ²⁶ Pamene Davide anafika ku Zikilagi , anatomiza vinangu pa vinthu vumene anapolola kunkhondo kuli akulu waku Juda , kuli abwenzi wake kunena kuti , "Onani , iyi mphaso yanu yachokela pa vumene tapokolola kuli wadani wa Yehova ." ²⁷ Anatomizako futi vinangu kuli azisogoleli waku Bethelo , nakuli waja wamene wanali ku Romothi yakumwela , na kuli waja wamene wanali ku Jottira, ²⁸ nakuli waja wanalimu Aroera , nakuli waja wanali mu Siphmothi , na kuli waja wanali mu Eshitemowa. ²⁹ Anatomizako futi vinangu kuli azisogoleli wamene wanali mu Rakali , nakuli waja wenzeli mumizinda yaku Jerahmeelayiti , na kuli waja wanali kumizinda yama kenayiti, ³⁰ na kuli waja wanali

mu Horoma , nakuli waja wanali mu Bori Ashani , nakuli waja wanali mu Athaki, ³¹ nakuli waja wenzeli mu Hebroni , na kumalo yonse yamene Davide eve mwine na masoja yake wanayenda kunkhalako.

Chapter 31

¹ Chinachitika kuti patapita izi pamene Amoni mwana mwamuna wa Davide enze ku kumbwila mulongo wake wamene sanabadwa naye wabwino wa ABisalomu wobadwa naye, winangu wabana bamuna ba Davide. ² Amoni anankala onzuzika paka anadwala chifukwa chamulongo wake Tama. Enze akali namwali, ndiye chinankala chovuta kuti Amoni achite chilichonse kuli iye. ³ Koma Amoni enze anli namunzake wamene zina yake ni Jonadabu mwana mwamuna wa Shimiya, mubale wa Davide. ⁴ Jonadabu anali mwamuna wanzelu zoipa. Jonadabu anakamba kuli Amoni kuti, "Nichani, mwana mwamuna wa mfumu, umanka unzuzi kuseni kuli konse? Nanga siuzaniuza?" Amoni anamuyanka iye kuti, Nikonda Tama, mubale wanga mulongosi wa Abisalomu." ⁵ Kuchoka apo Jonadabu anakamba kuli enve kuti, "gona po gona paku naku zipanga kwati wadwala. Pamene batate bako bazabwela kukuona, ubapempe kuti, "Nanga munganitiuzileko Tama mulongo eanga kuti anileteleko chintu chamene ningadye naku chipika pa menso panga kuti nichione nakudyela mumanja yake?" ⁶ PAmene apo Amoni ana gona nakuzipanga kudwala. Pamene ba mfumu bana bwela kumuona iye, Amoni anakamba kuli ba mfumu, "Napapata nitumileni mulongosi wanga Tama kuti anipangile vakudya pa vodwala vamga mumenso mwanga kuti nidye mu manja wake." ⁷ Pamene apo Davide anatuma mau kuli Tama kunyumba yake ya chifumu, kukamba kuti, "Yenda manje kunyumba ya Amoni mubale wako kuti ukamukonzele chakudya iye." ⁸ Pamene apo Tama anayenda kunyumba ya Amoni mubale wake kwamene enzeli gone pansi. Antenga vokandiwa va flaulo nakuvikonza naku panga mukate pamenso pake, nakupika. ⁹ Anatenga pani nakumupasila mukate iye, koma anakana kudya. chokonkapo Amoni anakamba nabantu benzemo kuti, "bachoseni bonse, muli ine." Pamene apo bonse banachoka mwamene enzelili. ¹⁰ Amoni anakamba kuli Tama kuti, "Leta vakudya muchipinda changa kuti tidye kuchokela mumanja yako." "Ndipo Tama anapeleka mukate wamene anabwela apanga, naku uleta muchipinda mwamubale wake Amoni. ¹¹ Pamene analeta chakudya kuli enve, anamugwila iye nakukamba kuli enve kuti, "bwela ugone naine, mulonga wanga." ¹² Anamuyanka iye kuti, "Iyayi, mubale wanga, usanipatikize sichifunika kuchitika mu Isilayeli. Usachite ichi chintu chonyansa! ¹³ NInga chose bwanji nsoni zanga? nanga iwe? uzankala moga umozi wavipuba mu Isilayeli manje napapata kamba na mfumu, pakuti sibaza kusunga kuchaka kuli ine." ¹⁴ Koma Amoni sanamunvelele iye, futi enzeli nampvu kuchila enve, anamugonjesa iye, nak gona naye. ¹⁵ Pamene apo Amoni ana zanda Tama nachi zondo chambili. Ana muzonda maningi iye kuchila nachilako chamene enze nacho pali enve. Amoni anakamba kuli enve kuti, "Nyamuka naku yenda." ¹⁶ Koma anamuyanka iye, "kuti, iyayi chifukwa cholakwa chachikulu cholengesa kuti niyende nichikulu kuchili vamene wanichita iye. ¹⁷ Mumalo mwake, anaitana wanchito wake naku kamba kuti, muchose mukzai kuchoka kuli ine, nakuvalako kuchiseko akachoka iye." ¹⁸ Kuchoka apo banchito bake banamuleta panja naku koma chiseko ata choka iye. Tama enzeli anavala chovala chopangiwa bwino chifukwa bana bakzi banfumu bana mwal benzeli ku vala sochabe. ¹⁹ Tama anafaka pulusa pa mutu pake naku ngamba chovala chake. Anafaka manja yake pa mutu naku chokako, ku mo kuwa pamene enzeli kuyenda. ²⁰ Abisalomu mubae wake anakamba kuli enve kuti, "Nanga Amoni mubale wako anali naiwe? Koma manje puzya, mulongo wanga Nimubale wako. Usachifakilile kumutima ichi." Ndipo Tama ansala eka munyumba yamu bale wake Abisalomu. ²¹ Koma pamene mfumu Davide anavinvela vonse ivi, anakalipa maningi. ²² Abisalomu sanakambe vili vonse kuli Amoni, pakuti Abisalomu enzeli kumuzonda chifukwa chavamene anabwela achita kuli iye namwamene anasebanyila Tama mulongo wake. ²³ Chinafika kuti panapita zaka zokwanila zibili pamene Abisalomu anankala nabo bosebesenza kudyesela mbelele ku Baal Hazo, yamene ili pafupi na Efram, Abisalomu anabaitana bonse bana bamuna ba mfumu kuti bamu tandalile kuja iye. ²⁴ Abisalomu anayenda kuli mfumu naku kamba, "Onani manje, wanchito wanu alina bodyesela mbelele. Napapata, kuti mfumu na banchito bake bayende naine, wanchito wanu." ²⁵ Ba mfumu bana muyanka Abisalomu, "Iyayi mwana wanga wamuna, Tizayenda tonse chifukwa tingankale vuto kuli iwe. "Abisalomu anapapata kuli mfumu, koma sana kwanise kuyenda, koma anamupasa madiliso yake." ²⁶ Chokonkapo Abisalomu anakamba kuti, "Ngati siso, nipempa kuti mubale eanga Amoni ayende naise." Apa ba mfumu banakamba kuli iye, "Nichifukwa chani chamene Amoni azayendaele naiwe?" ²⁷ Abisalomu anapitikiza Davide, ndiye anamuleka Amoni kuti nabonse bana bamuna bamfumu kuti bayenda naye. ²⁸ Abisalomu analamulila banchtio bake kukamba kuti, "Mvelani pafupi, pamene Abisalomu aza yamba kusokonezeka na vinyula napamene nizakamba kuli imwe kuti, kogesani Amoni, 'chokonkapo mumupaye iye. musankale boyopa. Nanga sina kulamulileni? Nkalani bolimba naku chenjala." ²⁹ Apa banchito ba Abisalomu banachita moga mwamene Abisalomu anaba lamulila kuti bachite. Kuchoka apo bonse bana bamuna ba mfumu bana nyamuka, ndipo mwamuna aliyense anyamuka nakukwela bulu yake baku taba. ³⁰ Chinachitika kuti, pamene benzeli bakali pa njila, pamene utenga unafika kuli Davide kukamba kuti, "Abisalomu apaya bana bamuna ba mfumu bonse, ndipo kulibe olo umozi asalako pali benve." ³¹ Chokonkapo mfumu inaimilila naku ngamba vovala vake, naku gona

pansi; Bonse banchito banaimilili pali iye navovala vongambika.³² Jonadabu mwana mwamuna wa Shima, mubale wa Davide, anayanka naku kamba kuti, "Lekani mbuya wanga asakulupilile kuti bana bafana bamuna banfumu bapaiwa, popeza kuti Amoni chabe eka ndiye Afa. Abisalomu anavi konza ivi kuchokela pasiku yamene Amoni anachita voipa kuli Tama mulongo wake.³³ Chaicho ichi chisalenge kuti mbuye wanga afakile ichi ku mutima, ngankale kukulupila bafa bamua bonse banfumu bafa, popeza Amoni eka ndiye afa."³⁴ Abisalomu anatba. Wanchito woyanganila ananyamula menso yake ndipo anaona bantu bambili babwela panja yalupili ya kumazulo kwamene enzelili.³⁵ Kuchoka apo Jonadabu anakamba kwa mfumu kuti, "Onani, Bana bamfumu bamuna ba bwela. Chili mongs mwamene wanchito wanu akambila."³⁶ Chinachitika kuti pamene anasiliza kukamb, bana bamfumu bamuna banafika naku lila mokwana. Mfumu nabonse banchito bake banalila kwakulu.³⁷ Koma Abisalomu anataba naku yendsa kuli Talmai mwana mwamuna wa Ammihud, mfumu ya Gesha. Davide enzekulila mwana wake mwamuna masiku yonse.³⁸ Pamene apo Abislomu anatba nakuyenda ku Gesha. kwamene anankala kwa zaka zitatatu.³⁹ Nzelu zanfumu Davide zinafunisisa kuyenda kumuona Abisalomu, popeza anatontola paza Amoni na infa yake.

Chapter 14

¹ Ndipo Yowabu mwana mwamuna wa Zeruia anaona kuti mutima wa mfumu ufunisisa kuona Abisalomu. ² Pamene apo Yowabu anatuma mau kuli Tekapri ndipo banauza mukazi wanzelu kuti amulete. Anakamba kuli iye, "Napapata uziapange munga ndiwe wachisoni naka vala vovala vachisoni. Napapata usasizozwe iwe mafuta, koma unkale munga mukazi wamene ankala wachisoni ntawi tali pabakufa. ³ Chokonkapo uyende kuli mfumu naku kamba aye pavintu vamene niza ku masulila." Pamene apo Yowabu anamu uza mau yamene azayenda kukamba kuli mfumu. ⁴ Pamene mukazi wochoka ku Tekoari anakamba na mfumu, anagoneka mutu wake pansi nakukamba kuti, "Nitandizeni ine." ⁵ Mfumu anakamba kuli, "Nichani chavuta?" Anayanka kuti, "Chazo ona nichakuti ndine mukazi wamasiye, bamuna banga banafa. ⁶ Ine, wanchito wanu, nenze nabana bamuna babili, benze kumenyana pamozi mu munda, ndiye kunalibe aliyense umozi obapatula benve. Umozi anatema winangu nakumupaya iye. ⁷ Manje munzi onse wanyamukila pa wanchito wanu, ndiye bakamba kuti, tipaseni mumanja mwatu mwamuna wamene gvesa mubale wake, kuti timu paye, kulipila mubale wake nabo baononge wopyana. Ati baza faka malasha yoshoka yamene nasiya, ndipo sibazasiyila bamuna banga zina kapena mibadwo pa ziko ya pansi." ⁸ Pamene apo mfumu anakamba namukazi kuti, yenda kunyumba yako, ine niza lamulila chintu chichitiwe pali iwe." ⁹ Mukazi waku Tekoria anabayanka ba mfumu, "mbuya wanga, mfumu, lekani kulakwa kunkala pali ine napali banja yanga. Mfumu namu pando wachifumu wake osalakwa." ¹⁰ Mfumu inayanka kuti, "Aliyense wamene azakamba chilichonse kuli iwe, umulete kuli ine, sazakugwilako futi." ¹¹ Chokonkapo anakamba kuti, Nipempa kuti mfumu iyitane munzeli Yehova Mulungu, kuti obwezela saza yenda pasogolo ku ononga aliyense. ¹² Kuchoka apo anakamba kuti, "Nipempa lekani kuti wanchito wanu apitilize kukambako mau kuli mbuya wake mfumu." Anakamba kuti, "Pitiliza kukamba." ¹³ Pamene apo mukazi anakamba kuti "Nichifukwa nichani munaganiza chintu chaso pa bantu ba Mulungu? ¹⁴ Popeza pokamba ichi chinut mfumu ilimonga mutnu wolakwa chifukwa mfumu sinabweze kunyumba futi mwana wake mwanu wamena anapishiwa. Popeza kuti tonse tifunika kufa, ndipo tili munga manzi yamene ta tiliwa pansi, yamene siyanga yolewe futi. Koma Mulungu sazatenga umoyo, mumalo mwake apeza njila yaba bamene bana pishiwa kuti ba bwelele. ¹⁵ Manje apa, kuona kuti nabwela kuakamba ici kuli mbuya wanga mfumu, nichifukwa chakuti bantu baniyofya ine. Wanchito wanu azikambisa paeka, 'Nizakamba manje na mfumu. Chizankala kuti amfumu bazachita kupempa kwa wanchito wabo. ¹⁶ Kapena mfumu izani mvelela ine naku chosa wanchito wake kuchokela mumanja mwa muna wamene anganiononge ine na mwana wanga mwamuna pamozi, kuchokela pa cholowa chamene Mulungu anatipasa. ¹⁷ Chokonkapo wanchito wanu anapempela, 'Yehova, Yehova, Nipempa kuti muleke mau ya mbuya wanga mfumu yoni pulumusa ponkala ngati mungelo wa Mulungu, nimwamene mbuya wanga mfumu alili pokamba chabwino kuchokela ku choipa. Lekani Yehova Mulungu wanu ankalale naimwe." ¹⁸ Kuchoka apo mfumu anayanka naku kamba kuli mukazi kuti, "Nipempa usanibise ine chili chonse chamene niza kufunsa." Mukazi anayanka kuti, "Lekani mbuya wanga mfumu ukambe manje." ¹⁹ Mfumu inakamba kuti, "sikwanja ya Yowabu yamene ili naiwe muli ivi vonse? Mukazi anayanka nakukamba kuti, "Pamene muli namyoy, mbuya wanga mfumu, kulibe wamene angatabe ku zanja lamanja kapena yakumazele kuonekela kuli vonse vamene mbuya wanga kuli akamba. Ni Yowabu wanchito wanu wamene anilamulila ine vintu vamene wanchito wanu akamba. ²⁰ Wanchito wanu Yowabu achitili ichi ku chinja masantuolidwe ya vamene vichitika. Mbuya wanga alina nzeli, munga nzeli zamu ngelo wa Mulungu, ndipo aziba vonse vamene vichilika mu zika." ²¹ Pamene apo mfumu anakamba kuli Yowabu kuti, "Ona manje, niza chita ichi chintu. Yenda kansi, ukamulete munyamata mongono Abisalomu abwelele." ²² Pamene apo Yowabu anagwesa mutu wake pansi muku lemekeza naku yamikila kuli mfumu, Yowabu anakamba kuti, lelo wanchito wanu aziba kuti apeza chisomo mu menso yangu, mbuya wanga, mfumu, muli ichi ya chita manga kupempa kwa nchito wake." ²³ Pamene apo Yowabu ananyamuka kuyenda ku Gesha, naku leta Abisalomu kumubweza ku Yelusalemu. ²⁴ Ba mfumu banakamba kuti, "Anga bwelele kunyumba yake, koma sanga one chinso changa." Pakunyumba kwake, koma sana one chinso cha mfumu. ²⁵ Manje mu Isilayeli kunalibe wamene enzeli kukambiwa ubwino kuchila pali Abisalomu. Kuchokela kutu kumo wakumendo kufikila kumwamba kumuntu kunalibe choipa pali enve. ²⁶ Ngati ajuba sisi zaka pakusila kwa chaka, chifukwa zinali zolema kuli enve, anali kuzipimisa sisi zake zinali kulema maskekeli yakwanila ngati 200 yamene yanali kupimiwa muchimo chachifumu. ²⁷ Kuli Abisalomu kuna badwa bana bamuna batatu na mukazi umozi, wamene zina yake inali Tama. Enzeli mukazi wabwini maninigi. ²⁸ Abisalomu anankala zaka tu zokwanila mu Yelusalemu, kopanda kuona chinso chamfumu. ²⁹ Chokonkapo Abisalomu anatuma mau kuli Yowabu kumutuma iye kuli mfumu, koma Yowabu sana bwele kuli iye. Ndiye Abisalomu anatuma mau kachibili, koma Yowabu sanabwelele nafuti. ³⁰ Abisalomu anauza banchito bake kuti, "Onani munda wa Yowabu ulipafupi na wanga, elo sama yendako kuja. Yendani naku ushoka." Pamene apo

banchito ba Abisalomu bana shoka minda. ³¹ Kuchoka apo Yowabu ananyamuka nakubwela kuli Abisalomu kunyumba yake, naku kamba kuli enve, "Nichani chamene banchito bako bashokela munda wanga?" ³² Abisalomu anayanka Yowabu kuti, ninatumiza mau kuli iwe kukamba kuti, "bwela kuti nikutume kuli mfumu kukamba kuti, "Nichani chamene nanachiokela ku Gesha? Sembe chankala chabwino kuti nikali kuja. Maje chaichi lekani nione chinso cha mfumu, elo ngati ndine wolakwa, lekani kuti benve bani paye." ³³ Pamene apo Yowabu anayenda kuli mfumu naku iuza. Pamene mfumu anitana Abisalomu, anabwela kwa mfumu naku belamisa pansi pamenso yamfumu, ndipo mfumu ina mupyopyosa Abisalomu.

Chapter 15

¹ Chinafika kuti patapita ivi pamene Abisalomu anakonzekela gareta na akavalo ba enve eka, naba muna bali fifite botamanga kusogolo kwake. ² Abisalomu enzeli ku ukakuseni naku imilila pambali yanji; a yoyenda ko ngennela kwa muzinda. Ngati mwamuna aliyense aliyense alina nkani ku bwela kuli mfumu kuti aweruze. ³ Ndipo Abisalomu enzeli kukamba kuli iye kuti, "Ona, nkani yako niyabwino nayo lungama, koma kulibe opasiwa mpavu naba mfumu kunvela nkani." ⁴ Abisalomu anapitiliza, "Asembe ninali namulilo mu ziko, kuti aliyense mwamuna wamene ali na mulandu wake kapena chifukwa chake abwele kuli ine, ndipo nizamupasa zachilungamo. ⁵ Chinachitika kuti ngati pamene aliyense mwamuna abwela kuli Abisalomu kumu lemekeza Abisalomu anali kuchosa kwanja nakumu kumbata iye naku mu myompyota. ⁶ Abisalomu anachita ivi kuma Isilayeli bonse bamene banali kubwela kuweluziwa kuli mfumu. Abisalomu anagwila mitima zabazimua bamu Isilayeli. ⁷ Chinachitika kuti pakusila kwa zaka folo pamene Abisalomu anakamba kuli mfumu kuti, "Nipempa kuti niyenda naku lipila kulumbila kwamene nina panga kuli Yehova mu Hebroni. ⁸ Pakuti wanchito wanu analumbila pamene ninali kunkala ku Gesha Arami, kukamba kuti, 'Ngati zo-onadi Yehova azanibweza ine futi ku Yelusalemu chokonkapo nizamutanda Yehova.'" ⁹ Pamene apo mfumu anakamba kuti, "Yenda mu mutendele." Pamene apo Abisalomu ananyamuka naku yenda ku Hebroni. ¹⁰ Koma chokonkapo Abisalomu anatuma bozanda muli zonse mutundu za Isilayeli. Kukamaba kuti, "Pamene chabe muzanvela chongo chalipenga, chokonkapo mukazembe kuti Abisalomu ndiye mfumu mu Hebroni." ¹¹ Naya Abisalomu kumayenda bazimuna bali 200 bochokela mu Yelusalemu, bamene bana itaniwa. Bana yenda mosaziba, Mosaziba vili vonse vamene Abisalomu anakonza. ¹² Pamene Abisalomu anali kupeleka nsembe, anaitana Ahitopelo kuchokela mumuzinda wake wa Gilo. Enzeli Mulangizi wa Davide. CHiwembu cha Abisalomu chinali cholimba, kukonka Abisalomu benzel ku pakilako. ¹³ Ntumwi anabwela kuli Davide kukamba kuti, "Mutima zaba zimuna mu Isilayeli za kanka pali Abisalomu." ¹⁴ Pamene apo Davide anakamba bamkuli bonse banchito bake bamene benzeli mu Yelusalemu naye kuti, "Nyamukani kulibe kapena umozi waise wamene azamutaba Abisalomu. Konzekani kuchoka manje, pakuti azati pitilila mwamusanga ise, ndipo azaleta ngozi pali ise nakuti menya mumuzinda na mpempeta ya lupanga." ¹⁵ Wanchito wa mfumu anakamba kuli mfumu, "Onani, banchito bako nibo konzeka kuchita vilivonse vamene mbuya wanga mfumu iza ganizaila." ¹⁶ Mfumu inayenda na banja yonse naye, koma mfumu anaiya bazikazi bali teni, bamene nalai bamai nini kuti basunge nyumba yachifumu. ¹⁷ Pamene mfumu anayenda nabantu bonse naye, banaimilila pa nyamba yosilizila. ¹⁸ Bankondo bake bonse banayenda naye, pali banayenda naye kunali ba Keretitisi, na bonse ba peletitisi, na bonse ba Gititisi-bazimuna bokwanila 600 bamene bana mukonka kuchokela ku Gati. ¹⁹ Chokonkapo mfumu inakamba kuli Ittai mu Gittiti, "Chifukwa nichani chamene uzatikonkela ise? Bwelela ukankale na mfumu, popeza ndiwe wachilendo nabo pita bwelela kumalo yako. ²⁰ Popeza kuti unachokako zulo nichani chamene nizakupangisa kuti uzi yenda chiyende yende konse konse naise? Siniziba ukatenge abale bako, chikondi chilonkazikika na chikulupililo viyende naiwe." ²¹ Koma Ittai anayanka mfumu anku kamba kuti, "Malinga Yehova ali wamoyo, na bwana mfumu yanga ali na moyo, nditi kumalo yali yonse kwamene bwana wanga mfumu azayenda, uko naye wanchito wanu azayenda kapena chitantaufa umoyo kapena kufa." ²² Davide anakamba kuli Itai, "Pitiliza kuyenda naise." Itai mu Gitite anapiliza kuyenda namfumu, pamozi nabazimuna bake na mabanja yake yonse yamene yanali naye. ²³ Ziko yonse inai mokwezeka mau pamene bantu benzeli kupita pamwamba pa chigwa yake Kidroni, na pamene mfumu ine yake inawoloka. Bantu bonse banyenda njila yaku chipululu. ²⁴ Na Zadoki nama Levitis bonse, monyamula likasa yachipangano cha Mulungu, banalipo. Bana faka likasa ya Mulungu pansi, chokonkapo Abiata anagwilisana bonse bapita kuchoka mumuzinda. ²⁵ Mfumu anakamba na zadoki kuti, Nyamula likasa ya Mulungu kubwelela mumuzinda. Ngati nizapapa chisomo mu menso ya Yehova, Azani bweza kuno ine naku nilangiza futi likasa napa malo pamene ankala. ²⁶ Koma ngati azakamba kuti, sindine wokondwela naiwe, onani, ndine pano, leka kuti achita kuli ine chamene chioneka chabwino kuli enve." ²⁷ mfumu inakamba futi kuli Zadoki wansembe kuti, "Nanga sindiwe miauli? Bwelela mumuzunda mwamu tendele nabana bako bamuna, Ahimaazi mwana wako mwamuna, na Jonatani mwana mwamuna wa Abiata. ²⁸ Ona nizalindila kuma fordhi ya Araba paka mau yaka choke kuli iwe kunizbisa ine." ²⁹ Pamene apo Zadoki na Abiata bana nyamula likasa ya Mulungu kuibweza mu Yelusalemu ndipo banankala kwamene kuja. ³⁰ Koma Davide anakwela kosoba nsapato kumendo naku lila pa mwamba pa mapili ya Olivi, ndipo anavininkila mutu wake aliyense mwamuna pali bantu bamene enze nabo anavininkila mutu wake, bana yenda pamwamba ndishi balila kwinangu bayenda. ³¹ Winangu anauza Davide kukamba kuti, "Ahitopelo niuzozi waba chiwembu alina Abisalomu." Davide anapempela, "Inu Yehova, sandisani malangi ya Ahitopelo kunkala upuba." ³² Chinafika kuti pamene Davide anafika pamwamba pa njila, pamene banaliku labila Mulungu Husai waku Arkiti anabwela ku kumana naye nachovala chake chongambika

namutu wake pa ziko. ³³ Davide anakamba kuli iye, ngati uzayenda naine, uzanivutisa ine. ³⁴ Koma ngiti uzabwelela ku muzinda naku kamba kuli Abisalomu kuti, 'Nizankala mwanchito wako, mfumu, monga mwamene nenzelili wanchito wa batate bako kudala, ndiye mwamene nizankalila wanchito wako, kuchoka apo uzasokoniza chilangizo xha Ahitopelo pamalo panga. ³⁵ Nanga suzankala na wansembe Zadoki na biata na iwe? chilichinse chamene anzanvela munyumba ya mfumu, ufunika ukaziuza Zadoki na Abiata wansembe. ³⁶ Ukaona kuti balinaba kuja bana babo bamuna, Ahimazi, mwana mwamuna wa Zadoki, na Jonatani, mwana mwamuna wa Abiata. Ukazituma vonse vamene wanvela mumanja mwao." ³⁷ Pamene apo Hushai, muzake wa Davide, anabwela mumuzinda pamene Abisalomu anafika naku ngena mu Yelusalemu.

Chapter 16

¹ Pamene Davide anapitilila pangono pamwamba pa lupili, Ziba wanchito wa Mepibosheti anamukumanya iye a abulu ovala chokwlelapo; pali benve penzeli mukate yokwanila 200, na vipaso va muzinga vili 200. ² Mfumu inakamba kuli Ziba kuti, "Nichani chamene waletela ivi vintu?" Ziba anayanka kuti, "Mabulu niya munyumba mwa mfumu yokwelapo, mukate zimina banu vakudya, vinyu niya aliyense wamene afoka kuti amwe muchipululu. ³ Amfumu bana banakamba kuti, "Nanga alikuti muzukulu mwamuna waba bwana bako?" Ziba anayanka kuti, "Onani, asala ka Yelusalemu, popeza akamba kuti, 'Lelo nyumba ya Isilayeli izabweza Ziko yaba tate banga kuli ine.'" ⁴ Kuchoka apo mfumu anauza Ziba kuti, "Ona, vonse vamene venze va Mepibosheti manje vankala vako." Ziba anayanka kuti, "Nazi chepesa kuli imwe, bwana wanga, mfumu lekani kuti nipeze chisomo mumenso mwanu." ⁵ Pamene mfumu Davide anamuyandikila Bahurimu, kuna choka panja mwamuna wochokela ku mutundu wa Saulo, wamene zina yake unali Shimi mwana mwamuna wa Gerai. Anachoka nakuyenda kwingu atembelela. ⁶ Anatema Davide myala naba kulu bakulu ba mfumu, ngankale kuti penze bankondo, naba kamalonda bamene benzeli kuzanja lamanja nakwa mazele kuli mfumu. ⁷ Shimi anaitana mwaku tembelela, "Yenda, choka kuno, muntu oyipa iwe, iwe mwamuna wamagazi! ⁸ Yehova abwezela bonse imwe pa magazi yamene munatila pakati pa banja ya Saulo, mumalo mwamene unalamulila. Yehova apasa munzi wako kuli mwana wako mwamuna Abisalomu. Waononge chifukwa ndiwe mwamuna wa magazi." ⁹ Chokonkao Abishai mwana mwamuna wa Zerua, anakamba kwa mfumu, "Chifukwa nichani iyi imbwa yakufa itembelela bwana wanga mfumu. Nuekeni niyenda naku juba mutu wake." ¹⁰ Koma ba mfumu banakamba kuti nichani chamene nizachita naiwe mwana mwamuna wa Zerua? Kapwena anitembelela chifukwa Yehova akamba naye kuti mulembele Davide, 'nindani utembelelea mfumu?" ¹¹ Pamene apo Davide anakamba kuli Abishai nabonse banchito bake, "Ona, mwana wanga mwamuna, wobadwa mutupi yanga, afuna kutenga umoyo wanga. Nivingati nanga vamene Benjamiti alakalaka kuonga moyo wanga? Mulekeni iye kuti atembelelewe, popeza Yehova amulamulila kuvichita. ¹² Kapena Yehova azayana pa chosayenela pali ine, nakunilipila ine na chabwino pakunitambela kake lelo." ¹³ Davide nabazi muna bake bana yenda pambali pake pambwamba paili, kwingu atembelela naku tila vidoti naku tema myala kuli enve pamene enze kuyenda. ¹⁴ Chokonkapo mfumu nabantu bonse bamene banali naye banalema, nfiye bana pumula pamene banaimilila usiku. ¹⁵ Koma za Abishalomu nabantu bonse ba zimuna bamu Isilayeli bamene banali naye, bana bwela ku Yelusalemu, naye Ahitopelo enzeli nabo. ¹⁶ China chitika kuti pamene Hushi mu Arkiti, muzake wa Davide, anabwela ku Abishalomu, kuti Hushari anakamba kuli Abishalomu kuti, "Mfumu inkale na moyo utali! mfumu inkale na umoyo utali! ¹⁷ Abishalomu anankamba kuli Hushari "Nanga ichi ndiye okulupiluka ku muzako? Nichani chamene sunayendelele naye?" ¹⁸ Hushari anakamba kuli Abisalomu kuti, "Iyayi; mumalo mwake, umozi wamene Yehova nabantu bake nabazi muna bamu Isilayeli basanka, ndiye kwamene niza satila, naku nizankala naye. ¹⁹ Futi, nimwamuna uti wamene niza sebenzela? Nanga siningasebenze pamenso pa mwana mwamuna wake? Monga mwamene nina sebenzela pamenso patate bake, niza sebenze pamenso pako." ²⁰ Chokonkapo Abishalomu anauza Ahitopelo, "Tipesko malangizo pali vamene tifunika kuchita." ²¹ Ahitopelo anayanka Abisalomu kuti, "Yenda kuli bakazi bakapolo bamene batate bana siyila ku sunga nyumba yachifumu, ndipo ba Isilayeli bonse bazaziba kuti wankala finga kuli batate bako. Chokonkapo manja yabonse bamene balina iwe yazankala yokosa." ²² Pamene apo bana yanzika hema ya Abishalomu pamwamba pa nyumba yachifumu, ndipo Abishalomu anayenda kuli bazi kazi baukapolo batate bake mu menso mwama Isilayeli bonse. ²³ Manje malangizo ya Ahitopelo muma siku yaja yanali monga mwamuna anvela kuchokela mukwama ya Mulungu mwine wake. Ndiye mwamene bonse na Abishalomu bana yaonela malangizo ya Ahitopelo bana ya onela.

Chapter 17

¹ Kuchoka apo Ahitopelo anakamba kuli Abisalomu kuti, "Apa amanje leka nisanke bazimuna bali 12000, ndipo niznyamuka naki tamangisa Davide usiku walelo. ² Nizabwela pali enve pamene ali wolema nakufoka naku muduitsa manta. ³ Bantu bamene balina enve baataba, ndiye niza menya mfumu yeka. Nizaleta bantu bonse kuli iwe monga mukazi wofuna kukwatila aletewa kuli mwamua wake, ndipo bantu bonse bazankala namutenelele pali." ⁴ Vamene Ahitopelo anakamba vina kondwelesa Abisalomu na bonse bosogoleli bamu Isilayeli. ⁵ Ndipo Abisalomu anakamba kuti, "Manje muyitaneni Hushi mu Arkuti, naye, tiyeni tinvele vamene azakamba." ⁶ Pamene Hushiri anabwela kuli Abisalomu, Abisalomu anamumasulila iye vamene Ahitopeleo anakamba nakufunsa Hushiri kuti, "Nanga tichite vamene Ahitopelo akamba? Ngati simwamene, tiuzevamene uza langiza." ⁷ Hushari anakamba kuli Abisalomu "malangizo yamene Ahitopelo akupasa ina ntawi siyabwino." ⁸ Hushari anapitiliza, "Uziba kuti batate bako na bantu babo bamuna nibankoma bolimba, ndipo nibo ukali, futi bali monga ka beeri kamene kapokewa tubana twake mu mumunda. Batate bako nibamuna bankondo, sibazagona naba nkondo usiku walelo. ⁹ Ona, apa manje abisama mumugodi kapena mumalo yenangu chingachitike kuti bazimuna bako bapaiwa pakuyamba kwa kumenyana kuti aliyense wamene azanvelako azakamba kuti kujubiwa kwatenga malo pali asilikali bamene bakonka Abisalomu. ¹⁰ Chokonkapo nabo bailikali bochenjela bamene mitima zabo zili monga nkalamu, bazayopa chifukwa bonse ba Isilayeli baziba kuti batate bako bamene ba mpavu, na bazimuna bamene alnaba nibo limba maningi. ¹¹ Nikulanga kuti onse ba Isilayeli babwelel pamozi kuli iwe, kuchokela ku Dani kufikila ku Beershiba, mmga mwaunyninji wamu chi enga zamene zili ku nyanja, nakuti yende kunkondo weka. ¹² Chokonkapo tiza bwela pali enve kuli konse kwamene angapezeke, naku muzunguluka monga mame yamene yagwela pansi. Sitiza siyako ngaklae umozi waba zimuna bake, kapena enve mwine wake, namoyo. ¹³ Ngati azabwelela mumuzinda, chokonkapo ba Isilayeli bonse bazaleta ntambo kumu zinda naku donsela mu manzi, paka kunkale kulibe olo kamwala kangono kopezeka kuja." ¹⁴ Ndipo Abisalomu nabazimuna bamu Isilayeli banakamaba kuti, "Malangizo ya Hushari mu Akuti yaliko bwino kuchila ya Ahitopelo." Yehova anazozza kukaniwa kwa langizo ya Ahitopelo yabwino kuti aletete chionongeko pali Abisalomu. ¹⁵ Chokonkapo Hushari anakamba luki ZAdoki na Abiata wansembe kuti, Ahitopelo alangiza Abisalomu nabazi sogoleli bamu Isilayeli umu na umu munjila, koma namu langiza vinangu. ¹⁶ Manje apa yenda mwamusanga iye, 'Usiku walelo musagonele ku ford ya Arabari, koma muyese ku tauka, ndaba mfumu izamelewa kufakako nabantu bonse bamene ili nabo.'" ¹⁷ Manje Jonathani na Ahimazi benze kunkala ku kasupe ka Rogeli. Wanchito mukazi enzeli kuyenda naku bauza vamene benze kufunika kuziba, popeza sibenze kufunika, kuonewa kuti bayenda mumuzinda. Pamene utenga unabwela, chokonkapo nikufunika kuyenda kuona mfumu Davide. ¹⁸ Koma mwamuna mufana anabaona pa ntawi iyi nakuyenda ku uza Abisalomu. Pamene apo Jonatani na Ahamai bana chokako mwamusanga naku bwela kunyumba ya mwamuna wina mu Bahurimu, wamene anali na chisime pakomo apke, ndiye pamene bana gwela. ¹⁹ Mukazi wamuna uyo anatenga vovininkila vapa chisime naku gweselapo mbeu pamwamba pake, kuti aliyense asazibe kuti Jonatani na Ahimazi bali muchisime. ²⁰ Bazimuna ba Abisalomu bana bwela kuli mukazi mwine wanyumba naku kamba kuti, "Ahimazi na Jonatani balikuti?" Mukazi anabauza kuti, "ba jumpe mumana." Pamene bana basakila konse konse naku sabapeza, bana bwelela ku Jerusalem. ²¹ Chinfika kuti pamene batapita Jonathani na Ahimazi bana chokamo muchisime. Banayenda ku uza mfumu Davide; Banakamba kuli eve, "Nyamuka mwamusanga ujumpe pamwamba pa manzi chifukwa Ahitopelo apasa ivi na aya malangizo pali iwe." ²² Kuchoka apo Davide anayamuka na bantu bonse bamene banali naye, ndiye bana kuwoloka mu jordani. kufikila kucha kwa kuseni kulibe kapena umozi wamene anakangiwa ku wolololka Jordani. ²³ Pamene Ahitopelo anaona kuti malangizo yake siya konkewa, anankala pali bulu yovala chonkalapoo nakuyenda kunyumba yake mumuzinda wake. Anakouza nyumba yake naku zimangilila anafa naku shikwa mumanda ya batate bake. ²⁴ Kuchoka apo Davidenanabwela ku mahanimu. Koma Abisalomu anaoloka Jordani, enve nabazi muna bonse bamu Isilayeli bamene banali naye. ²⁵ Abisalomu anafaka Amasa enzeli mwana mwamuna wa Jeta mu Ishimaliti wamene anayenda kuli Abigelo, wamene enzeli mwana mukazi wa Natashi na mulongo wa Zeruia, amai nake ba Yowabu. ²⁶ Kuchoka apo Isilayeli na Abisalomu mu banankala muziko ya Giliyadi. ²⁷ Chinachitika kuti pamene Davide anabwela ku Mahania mu, pamene Shobi mwana mwamuna wa Nahashi wochokela ku Rabai waba Amoniti, na Makiri mwana mwamuna wa Ammiel wochoka ku Lo Deba, na Bazillari mu Giliyadi wochoka ku Rogelimu, ²⁸ analeta vogoanapo navo vinikila, mabo nama poto, ²⁹ na uchi, bata, mbelele, meleki, kuti Davide na bantu bamene alinabo badye. Bazimuna aba banakamba kuti, "Aba bantu balina njala, nibolema na luzu muchipululu."

Chapter 18

¹ Davide anabapenda basilikali bamene banali nabo naku basanka bazisogoleli bali sauzande naba sogoleli bali handred pali benve. ² Chokonkapo Davide anatuma ba nkondo, anaba gaba muma gulu yatatu pali olamuliliwa kuli Yowabu, nama gulu yayatu yenangu pansu pali olamuliliwa kuli Abishari mwana mwamuna wa Zeruia, mubale wa Yowabu, nafuti yenangu magulu yayatu pansu pali kulamuliwa Itai mu Gititi. ba mfumu bana kamba ku bankondo kuti, "Zo-ona nazayenda naimwe, ine mwine wake." ³ Koma mwamuna anakamba kuti, "Musayenda ku nkondo, pakuti tikataba sibazatifakako nzelu ise, kapena bena baise bafa sibazafako nzelu. Koma mulingana nama sausande ya ise! chaicho chizankala chabwino kuti munkale okonzekela kuti tandiza ku choka mu muzinda." ⁴ Pamene apo mfumu inabayanka kuti, "Nizachita chilichinse chamene chioneka bwino kuli imwe." Mfumu anaimili pa chiseko chamuzinda pamene ba nkondo bonse benzeli kuchoka muma handredi nama sausande. ⁵ Mfumu analamuli Yowabu, Abisha, na Ita kukamba kuti, "muchite pagnono na munyamata wamene alina Abisalomu." Bantu bonse bananvela kuti mfumu yapasa bazisogoleli lamulo yake pali Abisalomu. ⁶ Pamene apo bankondo banayenda ku mbali ya ziko pa Isilayeli, nkondo ina zala munsanga ya Efram. ⁷ Bankondo bamu Isilayeli bana gonjesa kuja pamenso paba silikli ba Davide; kunali ku chekedwa kwa bazimuna bali twente sausande ija. ⁸ Nkondo ina zala konse ku mbali ya ziko ndipo bazimu bambili bamezewa na nsanga kudula na lupanga. ⁹ Chinachitika kuti Abisalomu ana kumanya ba silikali ba Davide. Abisalomu enzeli kuyenze bulu wake, ndiye bulu ina yenda pansu pantambi zikulu pamutengo wa oki ukulu, ndipo mutu waka unagwiliwa pa ntambi ya mutengo. Anasala alengela pakati pa kumwamba na pansu pamene bulu yamene enze kuyenza inapitiliza kuyenda. ¹⁰ Winangu anaona ichi naku uza Yowabu, Ona, Naona Abisalomu alelenga muutengo wa oki!" ¹¹ Yowabu anakamba kuli mwamuna wamene anamuza va Abisalomu kuti, "Ona!wanu ona! Nichani chamene suna ugwelese pansu? sembe naku pasa Mashekeli ya siliva na chiomanga mumusana." ¹² ¹³ Mwamuna anamuyanka Yowabu kutu, "Ngankale kuti nalandila mashekele yali sausanda ya siliva, siningafikise kwanja yanga pa mwana wanfumu, chifukwa tanvela tonse pamene mfumu akulamulilani iwe, kulibe wamene azagwila munyamata Abisalomu." Sembe naika umoyo wanga pa cha boza (ndiye kulib e chobisika kuchokela kuli mfumu). Sembe mwanilekelele ine." ¹⁴ Kuchoka apo Yowabu anakamba kuti, "sinizakuyembekezele iwe." Pamene apo Yowabu anatenga ntungo mumanja mwake naku ziponya pa mutima wa Abisalomu, pamene enzeli akali na moyo naku lelenga ku chokela mu mutengo wa oki. ¹⁵ Chokonkapo bamuna bafana bali teni bamene benze bana nyamula chida bana zunguluka Abisalomu, naku mumenya naku mupaya. ¹⁶ Chokonkapp Yowabu analiza lipenga, ndipo bankondo bana bwelela kuchokela kupilikisa a Isilayeli, popeza Yowabu anabwelesa bankondo bake. ¹⁷ Banamu tenga Abisalomu nakumu ponya muchimugodi chitali mu sanga; Bana shika tupi yake pause pamu mutolo ukuli wa myala, pamene a Isilayeli bonse bana taba, aliyense mwamuna kunyumba yake. ¹⁸ Manje Abisalomu, pamene enzeli na moyo, anabwela azimangila eka mwala ukulu ngati linga mu chigwa cha mfumu, popeza kuti anakamba, "Niliba mwana mwamuna wamene anganyamule kukumbukiliwa lowa zina yanga." Lunga anaipasa zina yake. kufikila na lelo imaitaniwa kuti chikumbuso cha Abisalomu. ¹⁹ Kuchoka apo Ahimazi mwana mwamuna wa Zadoki anakamba kuti, "Lekani ine nitamanga kuli mfumu yautenga wabwino, mwamene Yehova anamupulumusila kuchoka mumanja yaba dani bake." ²⁰ Yowabu anamuyanka kuti, "Suzankala onyamula utenga lelo, ukachite pa siku inango. lelo suzanyamula utenga chifukwa mwana wamfumu afa. ²¹ Chokonkapo Yowabu anakaba kuli mu Chushiti kuti, "Yenda, kauze mfumu vamene waona." Mu Cushiti anazichepesa kwa Yowabu, naku tamanga. ²² Ndipo Ahimazi mwana mwamuna wa Zadoki anakamba futi kuli Yowabu, "Chilichonse chamene chinga chitike, npiempa kuti nitamange naku mukonka mu Cushiti." Yowabu anayanka, "nichani chamene ufunila kutamanga, mwana wanga mwamuna, paku ona kuti suatenga mpaso iliyonse pa utenga?" ²³ "Chilichonse "chamene chizachitika," Ahimazi anakamba, "Nizatamanga." kuchoka apo Ahmazi anatamanga pa njila yaku dambo naku mupitilila mu Cushiti. ²⁴ Manje Davide enzeli nkale pakati pongenela napo chokela pachiseko. Kamalonda anayenda pamwamba pa utenga wapa geti wa dipa naku nyamula menso yake Pamene analangana anaona mwamuna achita kufika, atamanga eka. ²⁵ Kamalonda anakuwa naku uza mfumu, Kuchoa apo mfumu inakamba kuti, "Ngati ali eka, muli utenga mukamwa mwake. Wotamanga anabwela pafupi na mufupi namuzinda. ²⁶ Kuchoka apo kamalonda anaona winangu mwamuna atamanga, ndipo kamulonda anaitana wonkala pa geti; anakamba kuti, "Ona, kuli mwamuna winangu wamene atamanga eka." Amfumu banakamba kuti, "Naye aleta utenga wabwino." ²⁷ Pamene apo kamulonda anakamba kuti, "Niganiza monga kutamanga kwa mwamuna wamene ali pasogolo kuli monga kwa Ahimazi mwana mwamuna wa Zadoki. Amfumu banakamba kuti, "Nimwamuna wabwino ndipo abwela nautenga wabwino." ²⁸ Kuchoka apo Ahimazi anaitana aku kamba kuli mfumu kuti, "Zonse zili bwino," Anazi chepesa pamenso pa mfumu na nkope yake pansu naku kamba kuti "Adalisike azimua bamene bana nyamula manja yabo pali iwe bwana wanga mfumu." ²⁹

Pamene apo mfumu inayanka kuti, "Nanga zili bwino zonse na mwamuna mufana Abisalomu?" Ahimazi anayanka kuti, "Pamene Yowabu anituma ine, wanchito wanfumu kuli imwe, mfumu. naona kusokonezeka kwakulu, koma sininazibe kuti nichani." ³⁰ Chokonkapo mfumu anakamba kuti, zungulukia pambali naku imililia apa." Pamene apo Ahimazi anazunguluka naku fendela pambali, naki imilila. ³¹ Pamene apa mu Cushiti anafka naku kamba kuti, "kuli utenga wabwino wa bwana wanga mfumu, popeza Yehova akubwezelani lelo kuchokela kuli bonse bamene bana ku nyamukilani." ³² Chokonkapo mfumu anakamba kuli mu Cushiti kuti, "Nanga zili bwino namunyamata mungona Abisalomu?" Mu Cushiti anayanka kuti, "Badani ba bwana wanga mfumu, na bonse bamene bana kunyamukilani ku ononga imwe, bafunika kunkala monga mwamene uja munyamata alili." ³³ Kuchoka apo mfumu inankala nachisoni, nakuyenda ku malo pa mwamba pa geti naku lila maninigi pamene enzeli kuyenda analilia, "mwana wanga mwamuna, mwana wanga mwamuna Abisalomu! Bansembe nenze nafa ndine mumalo mwako, Abisalomu, mwana wanga mwamuna, mwamuna wanga mwamuna.

Chapter 19

¹ Yowabu anauziwa kuti, "Ona, amfumu balila naku dandaula pali Abisalomu." ² kugonjesa ika siku kunasanduka kulila pa bonse bankondo, pakuti bankondo banachinvela kuti chinakambiwa ija siku, amfumu banadandaula pa mwana wabo mwamuna." ³ Basilikali banachokapo mwazi zizi kuyenda mumuzinda ya siku, mange bantu bamene bannvela manyazi bamatabila pamene bataba kuchoka kunkondo. ⁴ Amfumu banavala pamenso pao nakulila naliu yapamwamba, "Mwana wanga mwamuna Absalomu, Abisalomu, Mwana wanga mwamuna, mwana wanga mwamuna!" ⁵ Chokonkapo Yowabu anageni munyumba muli mfumu naaku kamba kuli enve kuti, "Mwanivesa chisoni nkpo zaba silikali banu bonse lelo, bamene bapulumusaa umoyo wanu lelo, na umoyo wabana bamuna bany na wa bana bakazi banu, na myoyo zabazika bakapolo banu, ⁶ Chifukwa mukonda baja bamene bakuzondani, naku zonda baja bamene baki kondani. Lelo mwaonesi kuti asogoleli baba silikali naba silikali balibe mbali kuli imwe. Lelo nakululupila kuti ngati Abisalomu enze akali naumoyo, elo ise tonse tafa, icho sembe chaku kondwelesani. ⁷ Pa ichi manje nyamukani muyende panja naku kamba bwino kuli asilikali, pakuti nilumbila pali Yehobva, ngati simuzayenda, sipazankala kapena umozi mwamuna wamene azasala naiwe usiku uno. Ichi chizankala choipilako pali imwe kuchila ngozi zonse zamene zunakuchitikilaniponi imwe kuchokela pa unyamta wanu kufikila manje." ⁸ Pamene apo mfumu waimilila naku nkala pa get yamu muzinda ndiye banru bonse banauziwa kuti, "Onani, Amfumu bankala pa geti, "bantu bonse bana bwela pamenso pa mfumu. ⁹ Bantu bonse benze kushushana pabeka bamutundu yonse ya Isilayeli kukamba kuti, "Amfumu banati banati chosa ise kuchoka mumanja ya adani batu, nakuti pulumusa kuchoka mumanja mwaba Filistini, koma manje batabamo mu ziko chifukwa cha Abisalomu. ¹⁰ Abisalomu, wamene tinazoza pamwamba patu, afa ku nkondo. nanga nixhani chamene simukambapo vilivonse pazoleta amfumu?" ¹¹ Mfumu Davide anatumiza kuli Zadoki nakuli Abiata wansembe kukamba kuti, "kamba nabazi sogoleli baku Yuda kukamba kuti, "nichani mwankala osilizila kuleta mfumu kuti ibwelele kunyumba ya chifumu popeza kukamba kwama Isilayeli kupasa mfumu mwai, kuti babwezewe kunyumba ya chifumu? ¹² Ndimwe azibale banga, nyama yanga na fupa yanga. Nichani kansi chamene mwankalila bosilizila kubabweza amfumu?" ¹³ Kansi kamba na Amasai, "Nanga sindiwe wanyama yanga nafupa yanga? mulungu chitani naine, maninigi futi, ngati sindwe mukulu wasitima waba nkondokuchokela manje apo pamalo ya Yowabu." ¹⁴ Pamene apo anatengamitima yabazimuna bonse bamu Yuda ngati mwamuna umozi. Banatuma kuli amfumu kukamba kuti, "Bwelela, iwe naba zimuna bako." ¹⁵ Pamene apo mfumu inabwelelpo naku bwela ku Yodani. Manje bazimuna baku Yuda banabwela ku Giligo kuyenda kukumana na mfumu nakuti bailete mfumu uko ko Yodani. ¹⁶ Shimi mwana mwamuna wa Gela, mu Benjamiti wamene enzeli waku Bahurimu, anayendesa naba zimuna baku Yuda kuyenda kukumana na mfumu Davide. ¹⁷ Kunali bazi muna wani sausande naenve bochokela ku Benjamini, na ziba wanchito wa Saulo, na bana bake bamuna bali fiftini naba nchito benzeli na enve bali twenti. ¹⁸ Bana oloka Yodani mu menso mwamfumu. Bana oloka pakuleta banja ya mfumu nakuchita vonse vamene baganizila kuti ichi nixha bwini shimiri mwana mwamuna wa Gelai anazi chepesa pamenso pa mfumu akalibe kuyamba ku oloka Yodani. ¹⁹ Shimi anakamba kuli mfumu kuti, "Osati, bwana wanga, kunipezaa uchimwa kapena kuitana poganizila voipa vamene wanchito wanu anachita, siku yamene bwana wanga mfumu anachoka mu Yelusalemu. Nipempa, mfumu asachifake kumutima. ²⁰ Pakuti wanchito wanu aziba kuti analakwa. Onani, nichanifukwa chake nabwela lelo ngati oyambilila kuchokela muna banja yonse ya Yosefe kubwela kukumana na mwana wwanga mfumu." ²¹ Komo Abishiri mwana mwamuna wa Zeruia anayanka kuti, "Nanga Shimi apaiwa chifukwa kaichi, chifukwa anatembelela ozoza wa Yehova?" ²² Chokonkapo Davide anakamba kuti, "Nichani chamene nia chita naiwe, iwe mwana mwamuna wa Zeruia, kuti lelo wankala mudani kuli ine? Nanga aliyense mwamuna una azapaiwa lelo mu Isilayeli? Popeza siniza kuti lelo ndine mfumu pali Isilayeli?" ²³ Pamene apo mfumu anakamba kuli Shimiri kuti, "Suzafa." Mfumu inamu lonila iye nakulapa njazi. ²⁴ Kuchoka apo Mefibosheti mwana mwamuna wa Saulo. anabwela kukumana na mfumu. Senze anavala kumendo yake, kapena kujubako ndevu zake, kapena kuchapa zovala kuchokela pasiku pamene mfumu wachokapo kufikila siku yamene zinabwela kunyumba mu mutendele. ²⁵ Ndipo pamene anabwela kuchoka ku Yelusalemu kukakumana na mfumu, mfumu anakamba kuli enve kuti, "Nichani chamene sunayendelele naine, Mefibosheti?" ²⁶ Anayanka, "Bwana wanga mfumu, wanchito wanga anani nama, popeza ninakamba kuti, ' nizakwela pabulu vovala kuti niyende namfumu, chifukwa wanchito wanu niolemala. ²⁷ Wanchito wanga ziba ananiama ine, wanchito wanu, ku bwana wanga mfumu. Koma bwana wanga mfumu alimonga mungeli wa Mulungu. Chaicho, chitani chamene chili cha bwino mumenso yanu. ²⁸ Pakuti bonse bamunyumba mawa atate banga banali azimuna bakufa pamenso pa bwana wanga mfumu, koma munaika wanchito wanu pali abo bamene banadyela pa tebulo yanu. Nimpavu bwanji paichi zamene nili nazo kuti nipilize kulila kuli mfumu?" ²⁹ Kuchoka apo mfumu wakamba kuli enve kuti, "Nichani upiliza ku londolola?

Naganiza kuti iwe na ziba mu gabne minda." ³⁰ Pamene apo Mefibosheti anayatuka mfumu kuti, "inde, lekani atenge onse, popoza bwana wanga mfumu abwela kunymba yake mwamutendele." ³¹ Chokonkapo bazilai mu Giliditi anabwela kuchokela ku Rogilimu kuoloka Yodani na mfumu nakupelekeza mfumu pamwamba pa Yodani. ³² Manje Bazilai anali mwamuna nkalamba, na zaka zili 8. Anakonzekela mfumu navakudya pamene enze kunkala ku Mahanaimu, pakuti enzeli mwamuna wolemela. ³³ Mfumu anakamba kul Bazilai, " ³⁴ Bazilai anayanka amfumu kuti, "Nimasiku yangati yamene yasalako muzaka zaumoyo wanga, kuti niyende namfumu mu Yelusalemu? ³⁵ Nilina zaka 80. Ninga siyanise pali chabwino na choipa nanga? nanga wanchito wako angalabe vamene nimadya kapena vamene nimamwa? Ninga nvele futi boumba nanga? nichani chamene wanchtio wako okuvulisa kuli bwana wako mfumu? ³⁶ Wanchito wako azafuna kuti chabe ayendeko pamwamba pa Yodani na mfumu. Nichani chamene mfumu azanilapila nampoto ya so? ³⁷ Nipempa kuti lekani wanchito wanu abwelele kunyumba, kuti nikafele mumuzinda wanga pa manda ya tate naba mai banga. koma onani, uyo wanchito wanu Kimhamu. Lekani kuti awoloke na bwana wanga mfumu, naku chitila iw=ye chamene chioneka chabwino kuli imwe." ³⁸ Amfumu bana yanka kuti, "Kimhamu azayenda naine, ndipo nizamuchitila iwe, nachili chnse chamene ufunisisa kuchokela kuli ine, nizakuchitila ine." ³⁹ Kuchoka apo bantu bonse bana oloka Yodani, naba mfumu bana oloka, mfumu anapyopyosa Bazilali nakumu dalisa iye. Chokonkapo Bazilai anabwelela kunyumba yake. ⁴⁰ Pamene apo mfumu aalokela ku Giligo, Kimhamu naye anawoloka naye. Bankondo nonse baku Yuda banaleta mfumu, nabenangu bankondo bamu Isilayeli. ⁴¹ Mwamusanga azimua bamu Isilayeli banayamba kubwela kulimfumu naku kamba kuli mfumu kuti, "CHifukwa nichani azibale batu, ba zimuna bamu Yuda, banakubani naku kubweza mfumu na baja yake pa Yodani, na bonse bazimuna ba Davide naimwe?" ⁴² Pamene apo bazimuna bamu Yuda banayanka bamuna bamu Isilayeli kuti, "nichifukwa chakuti mfumu nimubululu watu wapafupi. Pali ichi? Nanga tadya chilichonse chamene mfumu ifunikila kulipila? Batipasako panso iliyonse?" ⁴³ Chokonkapo bazimuna bamu Isilayeli banayanka bazimuna baku Yda kuti, "Tili namitundu yokwanilamo teni yachibululu kuli mfumu, ndiye tilina ulamulilo wambili pali Davide kuchila imwe. Nanga nichani munati zondela ise? Nanga sikuvomeleza kwatu kuna yambililila kunveka kuti mfumu yatu ibwelele? Koma mau yabazi muna baku Yuda yanankala yaukali kuchila mau yaba zimuna bamu Isilayeli.

Chapter 20

¹ Kunachitika kuti kumalo yamene ayo yamozi kwenzeli mu ovuta wamene zina yake enzeli Shiba wamene mwamuna wa Bikiri, mu Benjamiti. Analiza lipenga naku kamba kuti, "Tilibe mbali muli Davide, kapena kunakala nachili chonse chloba muli mwana mwamuna wa Jesi. Lekani mwamuna aliyese ayende ku nyumba yake, Isilayeli." ² Pamene apo bonse bazimuna bamu Isilayeli banamutaba Davide naku konka Shiba mwana mwamuna wa Bikiri. Koma Bazi muna baku Yuda banakonka mfumu yabo pafupi, kuchokela ku Yodani kufikila ku Yelusalemu. ³ Pamene Davide anabwela ku nyumba yake yachifumu mu Yelusalemu, anatenga bazikazi bakapolo bali teni bamene anabwela asiya kuti basunge nyumba yachifumu, naku bafaka munyumba nakubalonda anali kubapasa vonse vofunikila, koma senzeli kugona nabo futi bana valizi wa kufikila masiku yakufa kwao, kunkala monga banali bofelewa. ⁴ Kuchoka apo mfumu inakamba kuli Amasai kuti, "Ifuna bazi muna bamu Yuda pamozi mumasiku yayatu; Ufunika kunkalapo pano, naiwe." ⁵ Pamene apo Amasai anayenda kutiana Yuda, Koma anachedwa kupitilila ntawi yamene ba mfumu bana mupasa iye. ⁶ Pamene apo Davide anakamba kuli Abishi, "manje Shiba mwana mwamuna wa Bikiri azati ononga maningi kupita namwamene Abisalomu anachita. Tenga banchita ba bwana wako, ba silikali banga nakumutangila iye, nangu bazapeza mizinda nakutiba." ⁷ Kuchoka apo bazi muna ba Yowabu bana mukonkamo mumbuyo, pamozi naba Keretiti naba Peletiti nabanonse bankondo bampavu. Bana siya Yelusalemu ku pilikishia Shiba mwana mwamuna wa Bikiri. ⁸ Pamene banali pachimwala chachi kulu chamene chiliku Gibiyoni, Amasai anabwela kukumana nabo. Yowabu enzeli vale chida chaba nkondo chamene anabwela avala, panali lamba mumusana mwake na ntuba mofakamo upanga. Pamene anayenda pasogolo, lupanga inagwa. ⁹ Pamene apo Yowabu anakamba kuli Amasai kuti, "nanga zili bwino naiwee, muswema wanga? Yowabu anatenga Amase mwkumugwila pandevu nakwanja yaku zanja lamanja kumu pyopyona iye." ¹⁰ Amasai sanaione fwaka yamene yenzeli kukwanja yaku mazela kwa Yowabu. Yowabu analasa Amasai mu malala ndiye matumbo yake yanatukila pansi. Yowabu sana mugwileko futi, Amasai anafa. ¹¹ Kuchoka apo umozi waba zimuna ba Yowabu anaimila pali Amasai, naku kamba kuti, "Iye wamene avomelezana na Yowabu, nawamene ali wa Davide, akonke Yowabu." ¹² Amasai anali kukunkuika muma gazi yake pakati pa njila pamene mwamuna anaona kuti bantu bonse bali imilile, ananyamula Amasai kuchoka munjila naku mufaka mumunda. Anamuponya nsalu pali iye chifukwa anaona bonse bana bwela kumuimilila. ¹³ Pamene bana muchosa munjila Amasai, Bonse bazimuna bana mukonkamo Yowabu, bonse bazimuna bana mukonkamo Yowabu mu pilikisha Shiba mwana mwamuna wa Bikiri. ¹⁴ Shiba anapita mumutundu yonse ya Isilayeli ku Abel Beti Maaca, naku mazijo yonse ya Bikiriti bamene bana bwela pamozi naju pilikisha Shiba. ¹⁵ Bana mugwila naku mu gonjesa iye mu Abel Beti Maaca. Bana manga njila yaku zinga pa muzinda ku chipupa. Bonse bazimuna bamene benzeli na Yowabu bana chi menya chipupa kuti bachi gwese. ¹⁶ Chokonkapo muzi mai wanzelu analila mwakukuwa mumuzinda, "Nvela, nipema anvela, Yowabu! Bwela pafupi naine kuti nakambe naiwe." ¹⁷ Pamene apo Yowabu anabwela pafupi naye, ndiye muzimai anakamba kuti, "Nanga ndiwe Yowabu?" Anayanka, "Ndine." Chokonkapo anakamba kuli enve kuti, "Nvela kumau ya wanchito wako, "Ninvela." ¹⁸ Kuchoka apo anakamba kuti, "banali kukamba muntawi yaku olala kuti, 'Zo-onadi funa malangizo ku Abeli, 'na malangizo ayo yaza siliza nkani." ¹⁹ Tili muzinda wamene uli wa mutendele maningi nabo kulupilika mu Isilayeli. uyesa kuononga muzinda wamene ni mai mu Isilayeli. Nichani chamene ufuna kumelela cholowa cha Yehova?" ²⁰ Pamene apo Yowabu anayanka naku kamba kuti, "Chinkale kutali, chinkale kutali naine, kuti nimele kapena kuononga." ²¹ Sicha zo-ona. Koma mwamuna wochokela kupili kuziko ya Efremu, otaniwa Shiba mwana mwamuna wa Bikiri, anyamula kwanja yake pa mfumu, Davide. Mupelekeni iye eke, ndipo niza nizamukochokamo kuchoka mu muzinda." Muzimai anakamba kuli Yowabu kuti, "Mutuu wake uzaponyewa kuli iwe pa chipupa." ²² Chokonkapo muzi mai anayeda kubantu bonse munzeli zake. Bana juba mutu wa Shiba mwana mwamuna wa Bikiri, naku uponya kuli Yowabu panja. Kuchoka apo analiza lipenga ndiye bazimuna bake bana chokamo mu muzinda, aliyense mwamuna kunyumba yake. Kuchoka apo Yowabu anabwelela ku Yelusalemu kuli mfumu. ²³ Manje Yowabu enzeli pamwamba pali bonse bankondo bamu Isilayeli, ndipo Benaia, mwana mwamuna wa Yehoiadai anali pamwamba pali bonse ba Kereti napali bonse ba Peletiti. ²⁴ Adoniramu enzeli pamwamba pali bazimuna bamene benze kuchitisa chitno zokakmiziwa, Jehoshafati mwana mwamuna wa AHiludi enzeli wolemba. ²⁵ Shiva enzeli mulembi ndiye Zodaki na Abiata benzeli bansembe. ²⁶ Irai mu Jairiti enzeli nduna ya mfumu.

Chapter 21

¹ Kunali njala muntawi ya Davide kwa zaka zitatu zokonkana, ndiye Davide anafuna funa nkope ya Yehova. Pamene apo Yehova anakamba kuti, "Iyi njala ili pali iwe chifukwa cha Saulo naba banja yake Yopaya, chifukwa anapaya ma Gibiyonites." ² Manje ma Gibiyonite sibenzeli ku chokela ku bantu baku Isilayeli: Benzeli ku chokela muli abo banasalako muli bama Amoriti bantu bamu Isilayeli banalapa njazi kuti sibaza bapya, koma Saulo anayesa kubapaya bonse, muchangu cha bantu ba Isilayeli na Yuda. ³ Pamene apo mfumu Davide anaitana pamozi ma Gibiyoniti naku kamba kuli benve kuti, "Nichani chamene mufuna niku chitileni? Ninga kutetezeni ba Yehova, bamene ba landila ubwino nanlongezo?" ⁴ Ma Gibiyoniti banamuyanaka iye kuti, "Sinjani ya siliva kapna golide pakati katu na Saulo kapena banja yake. chimozi mozi mwamene sichili kuli ise kupaya mwamuna aliyense mu Isilayeli." Davide anayanka kuti, "Nichani chamene mukamaba kuti niku chitileni?" ⁵ Bana yanka mfumu kuti, "Mwamuna wamene anayesa kutipaya ise tonse, wamene anachita chim=wembu pali ise, kuti tionogeke naku nkala tilibe malo mu malile ya Isilayeli- ⁶ bazimuna bali 7 mumibadwo mwake bapasiwe kuli ise, ndiye tizaba pachika pamenso ya Yehova mu Gibeia ya Saulo, yonskiwa na Yehova." pamene apo mfumu anakamba kuti, "Nizaku pasilani iwo kuli imwe." ⁷ Koma mfumu analekelela Mefiboshiti mwana mwamuna wa Jonathani mwana mwamuna wa Saulo, chifukwa chaku lumbila njazi kwa Yehova pakati kawo pakati ka Davide na Jonathani mwana mwamuna wa Saulo. ⁸ Koma mfumu anatenga bana bamuna babili ba Rizpa mwana mukazi wa Aia, bana bamuna bamene anabala kuli Saulo bana bamuna babili benze kuitaniwa Amoni na Mefiboshiti; Davide anatenga futi bana bamuna bali 5 ba Mirabi mwana mukazi wa Saulo, wamene anabala kuli Adrielo mwana mwamuna wa Bazilai mu Meholatiti. ⁹ Anabapasa mumanja mwama Gibiyoniti. Bana ba pachika palupili pamenso ya Yehova, ndipo banafa bonse pamozi bali 7. Bana paiwa mu ntawi yokoloa, mukuyamba kwamasitu yoyamba balele. ¹⁰ Kuchoka apo Rizpa, mwana mukazi wa Aia, anatenga novala va masaka nakuzi yanzikila mwine wake pa pili pambili yama tupi yokufa, kuchokela pakuyamba kwaku kololo kufikila pamene nvula inagwelapo kuchokela mu mwamba. Sana vomeleza tunyomi twa mu mwamba kuti tusokonze matupi muzuba kupena nyama zamusanga usiku. ¹¹ Chinauziwa kuli Davide vamene Rizpa, mwana mukazi wa Aia, mukazi kapolo wa Saulo, vamene anachita. ¹² Pamene apo Davide anayenda nakutenga mafupa ya Saulo nama fupa ya Jonathani mwana wake mwamuna kuchoka ku bazimuna baku Jabesi Giliyadi bamene bana bwela baba kuchokela malo yokumanilapo ya Beti Shani, kwamene ba Filisti bana ba pachika iwo, pambuyo pomupaya Saulo kuli ba Filisti mu Gilbo. ¹³ Davide anatenga kuchoka kuja mafupa ya Saulo nama fupa ya Jonathani mwana wake mwamuna, naku faka pamzi mafupa yaba muna bali 7 bamene bana pachikiwa, nabo. ¹⁴ Bana ika mafupa ya Saulo na mwana wake mwamuna mu zio ya Benjamin muzela ku manda ya Kishi tate wake. Bana chita vonse vamene mfumu inalamulila. Kuchoka apo Mulungu anayanka mapempelo yabo mu ziko. ¹⁵ Kuchoka apo ba Filisti banayenda kunkondo naba Isilayeli futi. Pamene apo Davide naba nkondo bake anayenda naku menyana naba Filisti. Davide anagonjesewa naku lema komenyana. ¹⁶ Ishi-Benobi, wamu midwo yabantu batali bampamvu wamene mukando wake wa bonzi anali kulema mashekeli yali 300, na wamene enzeli na chida na lupanga, anafuma ku paya Davide. ¹⁷ Koma Abishai mwana mwamuna wa Zeruia anapulumusa Davide, ana menya ma Filisti naku bapaya. Kuchoka apo bazimuna ba Davide banalumbila njazi kuli enve, kukamba kuti, usaka yendeko kunkondo naise futi, kuti usaka chose nyali ya Isilayeli." ¹⁸ Chinafika kuti pambuyo pochitika ivi kwenzeli futi nkondo naba Filisti ku Gobi, Pamene Sibejai mu Hushatiti anapya Safi, wamene enzeli umozi wa mibadwo ya Refiamu. ¹⁹ Chinafika futi munkondo naba Filisti ku Gobi, kuti Elhanani mwana mwamuna wa Jairi mu Bethlehemiti anapaya Goliati mu Gititi, ogwila nchito wamene mukondo wake unali monga mbali yamu kanjo. ²⁰ Chinafika futi munkondo inangu ku Gati kuti kwenzeli mwamuna mutali wamene eneli mwamuna navi kumo 6 pakwanja iliyonse navili 6 vikumo vaku mendo, pamozi venze twenti folo. Naenve anasika kuchokela ku Efaimu. ²¹ Pamene anavutisa Isilayeli, Jonathani mwana mwamuna wa Shimia, mubale wa Davide, Anamupaya. ²² Aba benzeli mibadwo za Refaimu waku Gati, ndipo bana paiwa namanja ya Davide na manja nyaba silika; i bake.

Chapter 22

¹ Davide anaimbila Yehova mau yanyimbo iyi pasiku yamene Yehova anamupulumusa iye kuchokela mumanja mwa ba dani bake, namu ma ja mwa Saulo. ² Anapempela, Yehova ni mwala wanga, tantwa langa, mupulumusi, wamene amani pulumusa ine. ³ Mulungu ndiye tanwe langa. Iye ndiye kotabila kwanga. Ndiye chikopa changa, nyanga ya chipulumuso changa, chitetezeo changa, nako tabila kwanga, iye wamene anandi amanichosa kuchokela ki nkanza. ⁴ Niza itana pali Yehova, wamene ayenela kumu tamanda, ndipo nipulumusiwa kuchoka kuli ba dani banga. ⁵ Pakuti mafunde ya imfa yanani zunguika ine, manzi yo tamanga ya chiongeke yanazininga ine. ⁶ Chingwe chaku Sheolo yananizi nguluka ine. Misampa ya infu inani valiza ine. ⁷ Muchisoni changa nina itana kuli Yehova; Nina itana kuli Mulungu wanga ananvele mau yanga kuchokela mutempele yake, naku itana kwangkuti anitandize kunyanda mumatu mwake. ⁸ Kuchoka apo ziko ina nyanganya naku njenjema. Maziko yaku mwamba yana njenjema ndipo yana nyanga nyisiwa, chifukwa Mulungu enzeli okalipa. ⁹ Chusi chinayenda mumwamba ku chokela mupuno mwake. Malasha yana yashiwa nayo. ¹⁰ Anasegu mumwamba nakubwela pansi, mpizi ikulu inali pansi pa mendo yake. ¹¹ Anakwela pa kerubi naku mbululuka. Anaonewa pama piko yachimpepo. ¹² Anapanga mfizi ngati hema mumbali mwake. Kufaka pamozi makumbi ya nvula ikulu mu mwamba. ¹³ Kuchokela kukaleza pamenso pake malasha yamulilo yanagwa. ¹⁴ Yehova anagunda kuchokela kumwamba. Wakumwamba mukulu anapunda. ¹⁵ Anautumiza mivi naku mwaza adani bake-kuyasha mpezi naku bamwaza iwo. ¹⁶ Kuchoka apo ngalande zamu nyanja zinaoneka; maziko ya muziko yosavala yanailaka pakuzuzula kwa Yehova paku chinga kwa kupema kwa mpuno zake. ¹⁷ Afaika pansi kuchokela kumwamba anamu gwila iye! ananichosa ine kuchokela mu manzi yalina mpavu. ¹⁸ Anani pulumusa ine kuchokela kuba dani banga ba mpavu, kuchokela kuli abo benze ba mpavu kuli ine. ¹⁹ Bana bwela pali ine pasiku ya chisoni changa, koma Yehova enzeli wonitandiza. ²⁰ Ananileta futi panja pamalo yoseguka maningi Ananipulumusa chifukwa enzeli wokondwela naine. ²¹ Yehova anipasa malipilo kulingana na chilungamo changa, Anibwezela ine kulingana naku yela kwa manja yanga. ²² Pakuti na sunga njila za Yehova, ndipo sinina chite voipa monga kusiya Mulungu. ²³ Pakuti kuweluza kwake kwa chilungamo kwenzeli pa menso panga, koma malemba ake, sininayachokemo. ²⁴ Ninali futi osalakwa pamenso pake, naku zisunga kuchoka ku chimo. ²⁵ Chaicho Yehova anibwezela ine kulinga namuyeso wachilungamo changa, ku malamulo yakuyela kwanga mumenso mwake. ²⁶ Kuli okulupilika mumazilangiza okukulupilika kwanu; kuli mwamuna wamene alibe choipa chili chonse, mumazi langiza osaipa chili chonse kwanu. ²⁷ kuli boyela mumazi langiza kuyrla kwanu, koma ndimwe boipa kuli ab boipa. ²⁸ Muma pulumusa bantu bonzunika, koma menso yanu siyafuna bozikweza, ndipo mumaba bweza pansi. ²⁹ Popeza ndimwe nyali yanga, Yehova. Yehova amayasha mudima wanga. ³⁰ Popeza pali imwe ninga tamange pali kuchinga apli Mulungu wanga ninga jumpe pamwamba pa chipupa. Koma Mulungu, njila zake nizangwilo. ³¹ Mau ya Yehova niyo yela. Ndiye chikopa cha aliyense wamene atenga kuchingilizwa muli enve. ³² Popeza nindani Mulungu kunja kwa Yehova, elo nindani mwala ukulu kumbuyo kwa Mulungu watu? ³³ Mulungu ndiye chochingiliza changa, ndipo amayenda bantu balibe choipa chili chonse munjila yake. ³⁴ Amapangisa mendo yanga yasanduka manga ya mbwalala naku mfaka pa mwamba pama pili. ³⁵ Amapunzisa manja yanga kumenya nkondo, na tukumo twanga kubendeka uta wansimbi. ³⁶ Munani pasa ine chozi chingilizila chakutumikila kwanu, kufafasa kwanu kwanipangisa kunkala mukulu maningi. ³⁷ Mwapanga malo yoseguka kuti mendo yanga yasatelele. ³⁸ Nina piliksha adani banga nakuba ononga. Sininabwelele paka naba ononga. ³⁹ Ninabasiliza nakuba pwanya; Sibanga nyamuke, Bagwa kumendo yanga. ⁴⁰ Mufaka mpavu pali ine manga lamba ya nkondo: Mufaka pansi panga aba bamene baninyamukila ine. ⁴¹ Munanipasa kumbuyo kwamukozi waba dani banga; Nina onogelatu baja bamene banali kunizonda. ⁴² Banalilila tandizo, koma kwenzelibe oba pulumusa. Banalila kuli Yehova, koma sanabayanke. ⁴³ Nina bamenya mutu gawo tungono tuli monga doti ya pansi, munaba ononga monga matika yamunjila. ⁴⁴ Munanichisa futi ine kuchokela muku yambana kwabantu banga mwani sunga ine ngati mukulu wama ziko. Bantu bamene sinenzo bana zipeleka kuli ine. ⁴⁵ Baku ziko yachilendo benze kupati kiziwa kuzi chepesa kuli ine. Pamene chabe banvela zaine, banani mvelela ine. ⁴⁶ Baku ziko yachilendo bana bwela na manta kuchokela kuzobagwilila. ⁴⁷ Yehova niwamoyo! Mwala wanga ukulu utamandike. Mulungu akwezekedwe, mwala ukulu wa chipulumuso changa. ⁴⁸ Uyu ndiye Mulungu wamene amaleta chilango chofukwa chaine, Iye wamene amaleta pasni bantu bamene bali pansi panga. ⁴⁹ Amandi masulu ine kuchokela kuba dani banga. zo-ona, munaninyamula kunifaka pamwamba pa abo bamene banani nyamukila ine. Munadi pulumusa kuchokela kubazimuna bachi wembu. ⁵⁰ Chaicho nizapeleka chiyamuko kuli imwe Yehova, pakati kama ziko; nizaimba matamando kuli zina yanu. ⁵¹ Mulungu apasa kupambana kukukulu kuli mfumu yake, naku langiza chipangano chokulupilika kuli azozewa wake, kuli Davide naku mibadwo yake muyayaya.

Chapter 23

¹ Manje aya ndiye mau yosilizila ya Davide- Davide mwana mwamuna wa Jesi, mwamuna wamene enze kulemekezewa, Umozi wamene anazozewa na Mulungu wa Yakobo, mwine wama Salimo yabwino. ² "Muzimu wa Yehova unakamba kupitila muli ine, na mau yake yenze pa lulimi yanga. ³ Mulungu wa Isilayeli anakamba naine, mwala ukulu wa Isilayeli anakamba kuli kuti, iye wamene alamulila molungama pa bazi muna, wamene alamulila mwaku yopa Mulungu. ⁴ Azankala monga kuwala kwa ku seni pamene zuba ya choka kuseni mwamene kulibe makumbi. Pamene mauzu yofewa ya Shuma pamwamba kuchoka pano kupitila mukuwala kwaka zuba pambuyo posila mvula. ⁵ Zo-ona, nyumba yanga sizankala choncho na Mulungu? Nanga sana panga chipangano chamuyaya naine, kulamulila nayo sungika munjila ili yonse naga safakilako kupumusiwa kwanga naku fikiliza zonse zofuna zanga? ⁶ Koma boipa bonse bazankala monga minga yamene ifunika kutaiwa. Chifukwa siyangaikiwe pamozi nakwanja imozi. ⁷ Mwamuna wamene avigwila afunika kusebenzesa chida cha nsimbi kapena chogwililako chankondo vifunika kushokewa pamene vili nkei." ⁸ Aya ndiye mazina yaba zimuna bampavu ba Davide: Josheb-Basshebeti mu Takemoniti, anali musogoleli waba zimuna bampamvu anapaya bazimuna bali 8 bandende ntawi imozi. ⁹ Kuchokela enve kwenzeli Elizera mwana mwamuna wa Dodi mu Ahohiti, imozi waba zimuna bampavu batatu. Anali na Davide pamene anagonjesa ma Filisiti bamene bana ba bwelela pamozi kuchita nkondo koma pamene bazimuna bamu Isilayeli bana bwela ba bwelela. ¹⁰ Eliazara anaimilila naku menyana nama Filisiti paka kwanja yake inalema naku gwilile kuli lupanga. ¹¹ Kuchoka enve kwenze Shama mwana mwamuna wa Agi, mu Harariti. Ba Filisiti bana bwela pamozi kwamene kunali munda wampoza, ndiye bankondo banataba. ¹² Koma Shama anaimilila pakati pa munda naku ichingiliza. Anabapaya ma Filisiti, ndipo Yehova anamuletela kupantana kwakulu. ¹³ Batatu mwaba silikali bali 40 banayenda kuli Davide pa utawi yokolola, ku kavu ya Aduilamu. bankondo bama Filisiti benze bana nkali ku chigwa cha Refaimu. ¹⁴ Pantaei ija Davide anali mu malo yobisamilamo, mu kavu, pamene Betetlehemu. ¹⁵ Davide enzo funisisia manzi ndipo anakamba kuti, "gati chabe umozi angani pase manzi kuchokela muchisime ku Betelehemu, chisime chamene chilipa gedi!" ¹⁶ Pamene apo aba bazimuna batatu bampavu banangena mubankondo baku ba Filisiti nak tapa manzi kuchokela mu chisime chamene chili pa gedi. Bana tenga manzi naku yaleta kuli Davide, koma anakana kuyamwa. Mumalo mwake, anayata panja kuli Yehova. ¹⁷ Kuchokela apo anakamba kuti, "Yehova, chinkale kutali naine, kuti nichite ichi. Nimwe manzi yabantu bamene bana pele myoyo zabo?" ndipo anakana kumwa. Ivi vintu vina chitiwa nabazi muna ba mpavu batatu. ¹⁸ Abshai, mubate wa Yowabu na mwana mwamuna wa Zeruia, enzeli musogoleli pa meamba paba tatatu. Anamenyanapo na mukondo naba zimuna bali 300 naku bapaya. Enze ku kukambiwa maningi naba silikali batatu. ¹⁹ Senzeli maningi ozibika ku chila aba batatu nanga? Anapangiwa oba sogolela koma, kuzibika kwake siku nafike pali kuzibika kwaba masilikali babatu bozibika maningi. ²⁰ Benaya wochoekla ku Kabzeda enzeli mwana mwamuna wa Jehoiadari; Anali mwamuna olimba wamene anachita vochta vampavu. Anapaya bana bamuna babili ba Arielo waku Mowabu. Anayenda futi pansu mumu godi naku paya nkalamu pamene yenzeli kuliza nkonono. ²¹ Kuchokela apo anapya mwamuna mukulu maningi waku Iguputo. Mu Iguputo enzeli na ndodo mumanja mwake, koma Benaya anamenyana chabe naye na mukondo. ²² Benaya mwana mwamuna wa Jehoidai anachita aya ma vampuvu, ndiye anapasiwa zina pamozi naba zimuna batatu bampavu. ²³ Anali opasiwa ulemu kuchila basilikali bonse pamozi bali 30, koma sanali kupasiwa ulemu kuchila bazimuna batatu bampavu. Koma Davide anamufaka kunkala woyanganila bama londa baka. ²⁴ Pabali 30 kwenzeli bazimuna aba: Asahelo mubale wa Yowabu, Elhanani mwana mwamuna wa Dodo kucjokela ku Betelehemu, ²⁵ Shama mu Haroditi, Elikai mu Haroditi, ²⁶ Helezi mu Palititi, Ira mwana mwamuna Ikeshi mu Tekoiti, ²⁷ Abieza mu Aratiti, Siberkari mu Hushatiti, ²⁸ Zalmoni mu Ahohiti, Maharai mu Netofatiti: ²⁹ Helebu mwana mwamuna wa Bannai, Mu Netafatiti, Itai mwana mwamuna wa Ribai kuchokela ku Gibeia kuba Benjamiti, ³⁰ Benaya mu Piratoniti Hidai waku chigwa cha Gashi. ³¹ Abi-Abon mu Abatiti, Azmaveti mu Bahumiti, ³² Eliaba mu Shalboniti, mwana mwamuna wa Jasheni, Jonathani mwana mwamuna wa Shama mu Harariti; ³³ Ahiamu mwana mwamuna wa Sharari mu Harariti, ³⁴ Elifeleti mwana mwamuna wa Ahasbai mu makatiti Eliamu mwana ³⁵ mwamuna wa Ahitopelo mu Giloniti. Hezroni mu Carmeliti, Parai mu Abitei, ³⁶ Igali mwana mwamuna wa Natani wochoekela ku Zoba, Bani wochoekela ku mutundu wa Gadi, ³⁷ Zeleki mu Amoniti, Nahari mu Berotiti, Armor bearer ku; i mwana mwamuna wa Zeruia, ³⁸ Ira mu Itriti, Garebu mu Itriti, ³⁹ Uria mu Ititi- 37 bonse.

Chapter 24

¹ Bafuti kukalioa kwa Mulungu kunabwela pali ma Isilayeli, ndipo kamba kuti, "Yenda, penda Isilayeli na Juda." ² Mfumu inakamba kuli Yowabu Mukulu waba nkondo wamene anali naye, "Yenda konse kumitundu ya Isialyel kufikila ku Beridhiba, naku penda bantu bonse, kuti nizibe baizmuna bonse pamoj bamene banga kwanise nkondo." ³ Yowabu anakamba kuli mfumu kuti, "Yehova Mulungu wanu Apakise bantu kali 100, na menso ya bwana wanga mfumu achione nichani bwana wanga mfumu afuna ichi?" ⁴ Koma, mau ya mfumu yenzeli yosilizila pali Yowabu na pali bazukulu ba nkondo. pamene apo Yowabu naba zukulu bankondo bana yenda kuchoka pamenso ya mfumu kupenda bantu ba Isilayeli. ⁵ Bana oloka Jodani naku nkala mufupi mwa Aroeri, mumuzinda wamu chigwa chaku mazulo kuchoka apo bamapitiliza kuyenda mu Gadi kufika ku Jaza. ⁶ Bana bwela ku Giliyadi baku ziko ya Tatimu Hodshiri, ku chokela apo kupitiliza kuyenda ku Dani Jani namu mbali kusogolo kwa Sidoni. ⁷ Banafika ku stronghold ya Tira, nayama Kenaniti. Chokonkapo bana yenda ku Negevu mu Yuda ku Beershiba. ⁸ Pamene bana yenda mu ziko yonse, bana bwelela mu Yelusalemu pakusila kwa myenzi ili nini nama siku yali 20. ⁹ Kuchoka apo Yowabu anabauza chibwelengelo chabonse bazimuna bandeo amfumu. Mu Isilayeli mwenzeli bali 800, 000 bolimbika dodansa lupanga, naba zimuna baku Yuda benzeli 500,000 baizmuna. ¹⁰ Chokonkapo mutima wa Davide unamuvuta pambuyo pobelenga baizmuna. Pamene apo anakamba kul Yehova kuti, "Nachimwa maningi pochita ichi. Manje, Yehova, tengani chimo manje yawa nchtio wanu, popeza nasobela mopusa maningi." ¹¹ Pamene Davide anauka kuseni, Mau ya Yehova yanabwela kuli muneneli Gadi, mulauli wa Davide, kukamba kuti, ¹² "Yenda ukakambe kuli Davide: 'Ichi ndiye chamene Yehova akamba: 'Nikupasa chonsaka pali vitatu. Sankapo chimozi pali ive.'" ¹³ Pamene apo Gadi anayenda kuli Davide nakukamba kuli enve kuti, "Pa zaka zitatu ko yanu ku kubwelelani muziko yanu? Kapena kutaba pamene adani bako baku pilikisha kwa myenzi itatu? olo kapena kukankale matenda pama siku yatatu? Manje ganiza yanko yamene niza bwelzela iye wamene anituma ine." ¹⁴ Kuchoka apo Davide anakamba kuli Gadi kuti, "Nili muvuto ikulu. Lekani tigwela mumanja ya Mulungu kuchila kuti tigwele mumanja ya mwamuna, popeza kuchita kwa chifundo chake nikwa kulu maningi." ¹⁵ Pamene apo Yehova anatumiza matenda pali Isilayeli kuchokela kuseni kufikila pantawi yokwanisika, bantu bokwanila 70,000 banafa kuchokela ku Dani kufikila ku Beershiba. ¹⁶ Pamene mungelo anafikisa kwanja yake pasogolo kuti aononge Yelusalemu, Yehova anachinja nzelu chifukwa cha kuononga kwamene chiza chia, ndipo anakamba ku mungeli wamene enzeli ku wononga bantu, "Kwasila! Manje bweza kwanja yako." pantawi imilile potwel pa Arauna mu Jebusiti. ¹⁷ Chokonkapo Davide anakamba na Yehova pamene anaona mungelo wamene anabwela anaponya matenda pa bantu, naku kamba kuti, "Nachimwa, 'Naku sobela mu mpulumpulu. Koma nkosa iyi, Nivi chani vamene zachita? Napapata lekani kwanja yanu ini lange ine na banga yaba tate banga!" ¹⁸ Kuchoka apo gadi anabwela siku ija kuli Davide nakukamba kuli enve kuti, "Yenda pa mwamba naku manga guwa ya Yehova potwela pa Arauna mu Jebusiti." ¹⁹ Pamene apo Davide anayende pamwamba monga Gadi anmu langiza kuti achitte iye, monga Yehova analamulila. ²⁰ Arauna anayanga panja naku ona mfumu naba nchito bake babwela. Pamene apo Arauna wayenda panja nakuzi chepesa kuli mfumu na nkope yake pansi. ²¹ Chokonkapo Arauna anakamba kuti, "Nichani bwanawanga mfumu abwelele kuli ine, wanchito wake?" Davide anayanka, "Kugula potwela, kuti nimange guwa ya Yehova, kuti matenda yachoke pa bantu," ²² Arauna anakamba kuli Davide kuti, "utenge ngati yanu, bwana wanga mfumu. CHitani nayo chamene chili chabwino mumenso yanu. Onani, aya ma oxani ya nsembe yoshoka navotwela nama goli ya nkuni. ²³ Vonse ivi, mfumu yanga, Ine, Arauna, nizaku pasani." kuchoka apo anakamba kuli mfumu kuti, "Yehova Mulungu wanu akuvomeleni imwe?" ²⁴ Mfumu anakamba kuli Arauna kuti, "Iyayi, nizaigula pamutengo siniza peleka ngati sembe yoshoka kuli Yehova chilichonse chamene sichinalipiliwe kali konse. Pamene apo Davide anagula potwela nama oxeni kwama shekeli yasiliva yalififite. ²⁵ Davide anamanga guwa ya Yehova kuja naku peleka nsembe yoshoka na nsembe yanu sonkano. Pamene apo Yehova anayanka pempelo pamalo pa ziko, na matenda pali Isilayeli yana lekeza.

1 Kings

Chapter 1

¹ Mfumu Davide anakota nakukala na zaka zambili, banamuvinikila nama blageti , koma eve sanamvele kufunda.

² Ba nchito bake banakamba kuli eve, "Tisakilile bwana watu mfumu musikana mungono wamene saziba

mwamuna. Amutumikile mfumu na kumusamalila eve. Agone mumanja mwake kuti bwana watu mfumu akale ofunda." ³ Ndipo beve bana sakila musikana okongola mukati mwa malile yonse ya Israeli. Beve banapeza Abishagi mu Shunammiti naku mupeleka kwa mfumu. ⁴ Musikana uyu anali okongola kwambili. Anatumikila mfumu nakumusamalila, koma mfumu sanamuzibe. ⁵ Pa ntawi ija, Adoniya mwana wa Hagiti anazikweza, anati, "Nizankala mfumu". Ndipo eve anakonzekela magaleta na apakavalo pamozi na amuna 50 kuti batamangile pasogolo pake. ⁶ Batate bake sibanamuvute, anati, "Ni Chifukwa chani wachita ivi kapena ivo?" Ndipo Adoniya anali muntu okongola maningi, obadwa pambuyo pa Absalomu. ⁷ Anakambilana na Joabu mwana wa Zeruya na wansembe Abiyatara. Ndipo bana mukonka Adoniya nakumutandiza eve. ⁸ Koma wansembe Zadoki, Benaya mwana wa Yehoyada, Nathani muneneli, Simeyi, Rei, na bamuna bampamvu ba Davide sanamukonke Adoniya. ⁹ Adoniya anapeleka nsembe ya nkosa, na ngombe, ngombe yamafuta pafupi na mwala wa Zohéleti, pafupi na Eni Rogeli. Anaitana abale bake bonse, bana bamuna ba mfumu, na bamuna bonse ba ku Yuda, banchito ba mfumu. ¹⁰ Koma sanayitane Nathani muneneli, Benaya, bamuna bampamvu, kapena Solomoni mubale wake. ¹¹ Pameneapo Nathani anakamba na Bathsheba mai wa Solomoni, kukamba, Kodi simunamvele kuti Adoniya mwana wa Haggithi ankala mfumu, ndipo Davide bwana watu saziba? ¹² Manje leka nikupase nzelu, kuti uzipulumuse weka na moyo wa mwana wako Solomoni. ¹³ Yendani kuli Mfumu Davide; mukambe naye, 'Bwana wanga mfumu, kodi simunalumbile kuli mutumiki wanu, na kuti, "Zoona Solomoni mwana wako azankala mfumu pambuyo panga, naku nkala pa mupando wanga wachifumu? Nanga bwanji Adoniya akulamulila?" ¹⁴ Pamene ukali kukamba na mfumu, ine nizabwela pambuyo pako ndipo nizasimikizila mau yako." ¹⁵ Ndipo Bathsheba anangena muchipinda cha mfumu. Mfumu anali okalamba kwambili, ndipo Abishagi mu Shunammiti ankatumikila mfumu. ¹⁶ Bathsheba anapepeza na kupasa ulemu ku mfumu. Pameneapo mfumu anakamba kuti, "Mufuna chani?" ¹⁷ Anakamba kuli eve, Bwana wanga, munalumbila kuli mutumiki wanu na Yehova Mulungu wanu, kuti, 'Zoona Solomoni mwana wako azankala mfumu pambuyo panga, azankala pa mupando wanga wachifumu. ¹⁸ Manje, onani, Adoniya ndiye mfumu, koma imwe bwana wanga mfumu simuziba. ¹⁹ Wapeleka nsembe za ngombe zambili, na ngombe zoyina, na nkghosa, ndipo ayitana bana bonse bamuna ba mfumu, wansembe Abiyatara, na Joabi mukulu wa ankhondo, koma sanayitane Solomoni mutumiki wanu. ²⁰ Pali imwe, bwana mfumu yanga, Aisraeli bonse ayangana pali imwe, kuti mubauuze wamene azankhala pamupando wanu wachifumu, bwana wanga. ²¹ Chamene chizachitika, pamene bwana mfumu yanga akasamila zanja na makolo ake, ine na mwana wanga Solomoni tizankhala ngati bakawalala." ²² Pamene eve anali kukamba na mfumu, muneneli Nathani anabwela. ²³ Ndipo anchito anauza mfumu, "Muneneli Nathani afika." Pamene eve anabwela pamanso pa mfumu, anawelama pamanso pa mfumu na nkhope yake pansi. ²⁴ Nathani anakamba kuti, "Bwana wanga mfumu, kodi munakamba kuti, 'Adoniya azankhala mfumu pambuyo panga, nakuankhala pa mupando wanga wachifumu?" ²⁵ Popeza lelo ayenda kupeleka nsembe ng'ombe zambili, zonenepa, na nkghosa. ndipo ayitana bana bamuna bonse ba mfumu, kazembe wa nkghondo, na Abyatara wansembe. Ba kudya na kumwa pasogolo pake, nakukamba kuti, 'Mfumu Adoniya ankhale na umoyo wautali!' ²⁶ Koma ine, wanchito wanu, wansembe Zadoki, Benaya mwana wa Yehoyada, na Solomoni wanchito wanu, sanatiyitaneko ife. ²⁷ Kodi bwana mfumu yanga mwachita izi kosatiuza, banchito banu, kuti nidani wamene azankhala pa mupando wachifumu pambuyo pake?" ²⁸ Pameneapo Mfumu Davide anayankha nati, "Niyitanilenikoni Bathsheba kuti abwele kuli ine." Eve anabwela pamanso pa mfumu ndipo anayimilila pamanso pa mfumu. ²⁹ Mfumu analumbila kuti, "Pali Yehova wamoyo, amene andiwombola ku mavuto yanga yonse, ³⁰ monga ninalumbila kuli imwe na Yehova, Mulungu wa Israeli, kuti, 'Solomoni mwana wako azankhala mfumu pambuyo panga, ndipo azankhala pamupando wanga wachifumu mumalo mwanga, 'Nizachita izi lelo." ³¹ Bathsheba anawelama mpaka nkhope yake pansi ndipo analemekeza mfumu nakukamba kuti, "Bwana wanga Mfumu Davide ankhale na umoyo osatha!" ³² Mfumu Davide anati, "Niyitanilenikoni Zadoki wansembe, Nathani mneneeli, na Benaya mwana wa Yehoyada." Beve banabwela kuli mfumu. ³³ Pameneapo mfumu nakamba kuti: "Tengani akapolo wa bwana wanu, ndipo mukwezeke mwana wanga Solomoni pa bulu yanga naku mupeleka ku Gihoni. ³⁴ Lekani Zadoki wansembe na Nathani mneneeli amuzoze ankhale mfumu ya Israeli nakuliza mapenga nakukamba kuti, Mfumu Solomoni ankhale na umoyo wautali!" ³⁵ Mwaichi muzabwela pambuyo pake, ndipo azabwela na nkunkhala pamupando wanga wachifumu. Namusankha kuti asogolele mfumu mumalo mwanga. Namusankha kuti ankhale musogoleli wa Israeli na Yuda. ³⁶ "Benaya mwana wa Yehoyada anayankha mfumu kuti, "Chinkhale sochabe! Lekani Yehova, Mulungu wa bwana mfumu yanga asimikizile izi. ³⁷ Monga Yehova ankhala na bwana mfumu yanga, chinkhale sochabe kuli Solomoni, nakupanga mupando wake wachifumu koposa wa bwana wanga Mfumu Davide." ³⁸ Pameneapo wansembe Zadoki, mneneeli Nathani, Benaya mwana wa Yehoyada, na Kerethiteshi na Pelethiteshi banayenda naku kwezeka Solomoni pa bulu ya Mfumu Davide; banamutenga ku Gihoni. ³⁹ Zadoki wansembe anatenga nyanga ya mafuta muchihema naku muzoza Solomoni. Pameneapo banaliza lipenga ndipo banthu bonse bana kamba kuti, "Mfumu Solomoni ankhale na umoyo wautali!" ⁴⁰ Pameneapo banthu bonse

banakwela patangu pake, ndipo banthu banaimba matolilo, na kukondwela na chisangalalo chachikulu; ndipo ziko inagwedezeke na phokoso zawo. ⁴¹ Adoniya na balendo bonse bamene banali naye banamvela pamene banasiliza kudya. Pamene Joabu anamvela kulila kwa lipenga anati, "Chifukwa nichani mu mzinda muli pokoso?" ⁴² Pamene anali kukamba, kunafika Jonathani mwana wa wansembe Abiyatara. Adoniya anati, genani, pakuti ndiwe munthu oyenela bwelesani uthenga wabwino." ⁴³ Pameneapo Jonathani anayankha Adoniya kuti, "Bwana wathu Mfumu Davide wayika Solomoni kunkhala mfumu, ⁴⁴ ndipo atumiza wansembe Zadoki, Nathani muneneli, Benaya mwana wa Yehoyada, ma Kerethitesi na Pelethitesi. Bana yenza Solomoni pa bulu yama mfumu Davide. ⁴⁵ Zadoki wansembe na Nathani mneneli anamuzoza kuti ankhale mfumu ku Gihoni, ndipo abwela kwameneuko alikusangalala, pakuti mu muzinda wonse wasanduka phokoso. Ndiye phokoso yamene mwamvela. ⁴⁶ Koma, Solomoni ankhala pamupando wachifumu. ⁴⁷ Ndiponso, banchito ba mfumu anabwela kudalisa bwana wathu Mfumu Davide, nakukamba kuti, Mulungu wanu apange zina ya Solomoni yopambana kuchila zina yanu, nakupanga mupando wake wacifumu upose mupando wanu wacifumu. ⁴⁸ Ndipo mfumu inagwada pansi pa bedi. Mfumu anakamba kuti, 'Alemekezeke Yehova, Mulungu wa Israyeli, wamene apasa lelo munthu wonkhala pamupando wanga wachifumu pasiku yalelo, na manso yanga yaona ichi.' ⁴⁹ Pamenepo balendo bonse ba Adoniya anachita mantha. Banayimilila ndipo aliyense anapita njila yake. ⁵⁰ Adoniya anayopa Solomoni, nakunyamuka, nakugwila nyanga za guwa ya nsembe. ⁵¹ Kenako anauza Solomoni kuti: "Adoniya ayopa Mfumu Solomoni, chifukwa wagwila nyanga za guwa yansembe, nati, 'Mfumu Solomoni anilumbilile kuti sazapaya mtumiki wake na lupanga.'" ⁵² Solomoni anakamba kuti, "Akazionesa ngati munthu oyenela, ngankhale sisi yake sizagwa pansi, koma ngati zoyipa zipezeke mwa eve, azafa." ⁵³ Pameneapo mfumu Solomoni anatuma banthu, bamene anabwelesa Adoniya pa guwa ya nsembe. Anabwela nakugwadila Mfumu Solomoni, ndipo Solomoni anakamba kuti, "Yenda kunyumba kwako."

Chapter 8

¹ Pamenepo Solomo anasonkanisa bakulu ba Israyeli, na bonse basogoleli ba mitundu, na basogoleli ba mabanja ya bana ba Israyeli, pamenso pake ku Yerusalemu, kuti akabwelese likasa ya chipangano cha Yehova kuchokela ku Mizinda ya Davide, ndiyo, Ziyoni. ² Bamuna bonse ba Israeli banasonkana kwa Mfumu Solomoni ku madyelelo, mumwezi wa Etanimu, wamene ni mwezi wachisanu namba seveni. ³ Bakuluakulu bonse ba Israeli anabwela, na bansembe bananyamula likasa. ⁴ Bananyamula likasa la Yehova, mutenti yokumanilamo, na vopangiwa vonse vopatulika vamene vinali mutenti. Bansembe na Balevi banabwelesa izi. ⁵ Mfumu Solomoni na bosonkana bonse ba Israeli banasonkana pasogolo pa Likasa, kupeleka nkosa na ng'ombe zamene sibanakwanise kuzipenda. ⁶ Bansembe banangenesa likasa la chipangano cha Yehova kumalo yake, ku chipinda chamukati cha munyumba, Malo yoyela yopambana, pansi pa mapipiko ya Akerubi. ⁷ Chifukwa Akerubi banatambasula mapipiko yawo kumalo kwa Likasa, na kuvininkila Likasa na mitengo yake yonyamulila. ⁸ Mitengo inali itali kwambili chakuti kosilizila kwake yanali kuonekela kuchokela kumalo yoyela kusogolo kwa chipinda chamukati, koma siyanali kuonekela panja. yalipo mpaka lelo. ⁹ Munalibe kantu mulikasa koma chabe minyala ibibli yamene Mose anaikamo ku Horebe, pamene Yehova anapanga chipangano na bana ba Israyeli, pamene banachoka muziko ya Aigupto. ¹⁰ Panali kuti pamene bansembe banachoka mu malo yopatulika, kumbi inazula mu tempele ya Yehova. ¹¹ Bansembe sibanakwanise kuimilila chifukwa cha kumbi, chifukwa ulemelelo wa Yehova unazula mu nyumba yake. ¹² Pamenepo Solomoni anati, "Yehova akamba kuti azankala mumtima otikama, ¹³ koma nakumangila malo, malo yako yonkalamo muyayaya." ¹⁴ Ndipo mfumu inapindamuka na kudalisa bonse mupingo wa Israyeli, pamene mupingo bonse wa Israyeli unali woimilila. ¹⁵ Anakamba kuti, Alemekenzeke Yehova Mulungu wa Israyeli, wamene anakamba na Davide tate wanga, na kukwanilisa na manja yake, kuti, ¹⁶ Kuyambila siku yamene ninachosa bantu banga Israyeli mu Aigupto, sininasanke muzinda kuchoka mumitundu yonse ya Israeli kuti amange nyumba, kuti zina yanga linkale pamenepo. Mwaichi, ninasankha Davide kuti alamulile banthu banga ba Israeli. ¹⁷ Manje chinali mumutima wa Davide tate wanga ndi mtima womangira nyumba dzina la Yehova Mulungu wa Israyeli. ¹⁸ Koma Yehova anati kwa atate wanga Davide, Popeza munali mumutima mwanu kuti mumange nyumba pa zina yanga, munachita bwino kuli ichi mumutima mwanu. ¹⁹ Koma iwe suizamanga nyumba; Mumalo mwake, mwana wako wamwamuna, wamene azakabadwa mumusana mwako, azakamanga nyumba pa zina yanga. ²⁰ Yehova wakwanilisa mawu yamene anakamba, chifukwa nanyamuka mumalo mwa Davide batate banga, ndipo ninkala pamupando wachifumu wa Israyeli, monga Yehova anakamba. ²¹ Namanga nyumba mu zina ya Yehova, Mulungu wa Israyeli. Napanga malo ya likasa kwamene kuja, mwamene muli chipangano cha Yehova, chamene anapangana na makolo bathu pobachosa muziko ya Aigupto. ²² Solomoni anaimilila pasogolo pa guwa ya bansembe ya Yehova, pamenso pa banthu bonse ba Israyeli, natambasulira manja ake kumwamba. ²³ Iye anati, "Yehova, Mulungu wa Israeli, palibe Mulungu wina monga imwe kumwamba kapena pansi pano wamene amasunga chipangano chake na bakapolo banu bamene bamayenda pamenso panu na mutima wabo bonse; ²⁴ Imwe bamene mwasunga pamozi na mutumiki wanu Davide batate banga, vamene munamulonjeza. Zoonu, munakamba na kamwa kanu ndipo mwakanilisa na kwanja kwanu, monga chili lelo. ²⁵ Manje, Yehova Mulungu wa Israyeli, chitani zamene munalonjeza mutumiki wanu Davide tate wanga, pamene munakamba kuti, Siuzasoba kunkala na muntu pamenso panga wakunkala pa mupando wachifumu wa Israyeli, ngati chabe bana bako basamala mu kuyenda pasogolo panga, monga wayendela pasogolo panga. ²⁶ Manje, Mulungu wa Israyeli, lekani mau yanu yasimikizike, yamene mwayakamba kuli Davide mutumiki wanu tate wanga. ²⁷ Ushe Mulungu nizoona azankala paziko lapansi? Onani, thambo yonse na kumwamba sikungankhale kukukwanisani imwe-nanga kuli bwanji kwa iyi tempele yamene namanga! ²⁸ Ndipo lemekezani pempelo ya mutumiki wanu na kufuna kwake mozichepesa, Yehova Mulungu wanga; nvelani kulila na pempelo yamene mutumiki wanu apempela pamenso panu lelo. ²⁹ Lekani Menso yanu yankhale yoseguka pali iyi tempele usiku na mu kukachisi uyu usiku na muzuba, kumalo yamene mwane kuti, Zina langa na kunkhalapo kwanga kuzankhala kwamene kuja, kuti mumvele mapemphelo yamene mutumiki wanu azapemphela pali yano malo. ³⁰ Sopano mvelani pempelo yozichepesa ya mutumiki wanu na banthu banu ba Israeli pamene tikupemphela pamalo yano. Zoonu, mvelani kuchokela kumalo kwamene munkala, kuchoka ku mwamba, ndipo mukavela, kululukilani. ³¹ Munthu akachimwila munzake wapafupi na akufunika kulapila chipangano, ndipo ngati abwela na kulapila chipangano pasogolo pa guwa yanu yansembe munyumba ino, ³² mvelani kuchokela kumwamba na kuchita kantu. Weluzani bakapolo banu, kuweluzi wosalungama na kuleta zamene achita pamutu wake. Muzikamba babwino kuti wosalakwa na kumupasa monga mu kuyela kwake. ³³ Pamene banthu bako ba Israeli bagonjesedwa kuli badani chifukwa bakuchimwilani imwe, ngati batenukila kuli imwe, kukambilila pa zina yanu, nakupempela, nakufuna ubwino wanu mu tempele ino- ³⁴ napapata nvelani

kuchoka mumwamba na kukulukilila uchimo wa banthu banu ba Israeli; babweleseni futi kumalo yamene munapasa makolo yawo.³⁵ Pamene thambo yavalika ndipo kulibe mvula chifukwa banthu bakuchimwilani — ngati bapemphela bakalangana pamalo yano, kukamilila pa zina yanu, na kuchoka ku machimo yawo pamene mwabavutisa-³⁶ pamenepo mvelani kumwamba na kukulukilila chimo ya mutumiki wanu na banthu banu ba Israeli, pamene mwabapunzisa njila yanu yabwino yamene bafunika kuyendamo. Tumani nvula pamalo yanu, yamene mwapasa kuli banthu banu monga cholowa chawo.³⁷ Tiyelekeze kuti muziko mwanu muli njala, kapena ngati muli matenda, chimphepo kapena kachilombo, zombe kapena malasankhuli; kapena kuti ngati mudani aukila zipata za muzi muziko yao, kapena kuti pali mulili uli wonse kapena matenda;³⁸ ndipo nichani ngati mapemphelo na zopempha zichokela kwa munthu, kapena na banthu banu bonse ba Israyeli, ali bonse aziba mulili wamene uyo mumutima mwake; atambasula manja yake kuyangana ku tempele iyi.³⁹ Ndipo mvelani kuchokela kumwamba, kumalo kwamene munkala, khululukilani na kuchitapo kanthu, ndipo bwezelani munthu aliyense pali vonse vamene achita; muzina mutima wake, chifukwa imwe ndipo imwe chabe muziba mitima ya bonse banthu.⁴⁰ Chitani izi kuti bakuyopeni masiku yonse yamene bazankhala mu malo yamene munapasa makolo yawo.⁴¹ Komanso mulendo wonkhala pakati pa banthu banu ba Israeli: bakabwela kuchokela ku ziko yakutali chifukwa cha zina lanu,⁴² chifukwa bazamvela za zina yanu yaikulu, na zanja yanu yamphamvu, na mukono wanu wokwezedwa, pamene babwela na kupemphela kuyangana ku tempele iy,⁴³ napapata mvelani kuchokela kumwamba, kumalo kwamene munkala, na kuchita chilichonse chamene mulendo akupempani imwe. Chitani ichi kuti banthu bonse paziko lapansi bazibe zina yanu na kukuopani, monga mwamene mumachitila banthu banu ba Israeli. Chitani ichi kuti bazibe kuti nyumba iyi yamene namanga iyitaniwa pa zina yanu.⁴⁴ Tiyelekeze kuti anthu anu apita kukamenyana na mudani, kudzera njira iliyonse yomwe mungatumize, ndipo akuganiza kuti akupemphera kwa inu, Yehova, kumzinda umene mwasankha, komanso kunyumba imene ndamangira dzina lanu.⁴⁵ Kenako mverani kumwambako pemphero lawo ndi pempho lawo, ndipo athandizeni pa zomwe akuchita.⁴⁶ Tiyelekeze kuti bakukuchimwilani, popeza palibe wamene samachimwa, ndipo muganiza kuti mwabakwiyila nakubapeleka mumanja mwa badani, kotelo kuti mudani wamene uyo azabatenga ukapolo kuziko yawo, ngakhale kutali kapena pafupi.⁴⁷ Ndiye ganizilani kuti bakumbukila kuti bali muziko yamene banatengewa ukapolo, nakuganiza kuti balapila nakupempha chifundo kwa imwe kuchokela kuziko ya bamene banabatenga. Tiyelekeze kuti banakamba, Tachita zolakwa ndipo tachimwa. Tachita vinthu voipa.⁴⁸ Tiyelekeze kuti abwelela kwa inu na mitima yabo bonse na moyo wabo bonse mu ziko ya badani bawo bamene banabapoka, ndipo ngati bapemphela kwa imwe kusata ziko yawo, yamene munapasa makolo yawo, na muzinda wamene munausankha, na kunyumba yamene ndamangamo zina yanu.⁴⁹ Pamenepo kuchokera kumwamba, kwamene imwe munkala, mvelani imwe pemphero yabo na chopempha chabo kupempha tandizo, ndipo muzabalungamisa.⁵⁰ Mukululukire banthu banu bamene banakuchimwirani, na volakwa vawo vonse vamene banakulakwirani, ndipo mubachitire chifundo pamenso pa bamene bawagwira, na kubachitira chifundo bamene banabagwira.⁵¹ Iwo ni banthu banu bamene munabasankha, bamene munawapulumutsa ku Iguputo ngati kuti mukuwotcha chitsulo.⁵² Maso anu yakhale otsegukila pempho la ine mtumiki wanu, na zopempha za banthu banu Israyeli, kuti muwamvere iwo, pamene iwo alira kwa inu.⁵³ Pakuti munawapatula pakati pa anthu a mitundu yonse ya paziko lapansi yankhale banu, na kulandila malonjezano anu, monga umo munalongosolela na Mose mtumiki wanu, m'mene munaturutsa makolo athu m'Aigupto, Ambuye Yehova.⁵⁴ Ndipo kunali pamene anasiliza Solomoni kupemphela pemphelo ili lonse ndi kupemphera kwa Yehova, anauka pasogolo pa guwa la nsembe la Yehova, atagwada pansu, ndi manja ake atatambasulira kumwamba.⁵⁵ Iye anayimirira ndi kudalitsa mpingo wonse wa Israeli mofuwula,⁵⁶ nati, "Alemekezeke Yehova, amene wapatsa anthu ake Aisraeli mpumulo mwa kusunga malonjezo ake bonse. Palibe mawu amodzi omwe sanakwaniritsidwe pa malonjezo onse yabwino ya Yehova na Mose mutumiki wake.⁵⁷ Lekani Yehova Mulungu wathu ankhale naife monga anachitila na makolo bathu.⁵⁸ Asatisiye kapena kutitaya, kuti atembenukile mitima yathu kwa iye, kuti tikonke njila zake zonse, na kusunga malamulo yake, na malemba yake, yamene analumulila makolo yathu.⁵⁹ Vomelezani mawu aya nakamba, yamene napempha pamenso pa Yehova, yankale pafupi na Yehova Mulungu wathu usana na usiku, kuti atandize pa nchito ya mutumiki wake na mulandu wa anthu ake Israyeli, monga zifunikila siku na siku;⁶⁰ kuti anthu onse ya ziko lapansi bazibe kuti Yehova ndiye Mulungu, ndipo palibenso Mulungu wina;⁶¹ Potero mutima wanu ukhale wokhulupirika kwa Yehova Mulungu wathu, kuyenda mumalemba ace, ndi kusunga malamulo ake, monga lero."⁶² Mwaichi mfumu na bonse Israeli bonse pamozi naye anapeleka nsembe kwa Yehova.⁶³ Solomo anapereka nsembe yoyamika kwa Yehova: ng'ombe zikwi makumi awili mphambu zibili, na nkhusa 120,000. Momwemo mfumu na bana bonse ba Israyeli banapatula nyumba ya Yehova.⁶⁴ Pa siku yamene iyo mfumu inapatula pakati pa bwalo pasogolo pa tempele ya Yehova; pakuti pamenepo anapeleka nsembe zopseleza, na nsembe za mbeu, na mafuta ya nsembe zoyamika; zing'onozing'ono kulandila nsembe yopseleza, nsembe yambewu, ndi mafuta a nsembe zoyamika.⁶⁵ Pamenepo Solomoni anachita madyelelo pantawi yamene iyo, naba

Israyeli bonse nayeve, musonkano waukulu, kuyambila ku Lebano Hamati kufikila ku musinje wa Aigupto, pamenso pa Yehova Mulungu wathu masiku yali seveni na yenangu masiku yali seveni, pamozi nimasiku yali fotini. ⁶⁶ Pa siku lachisanu na chitatu anabatuma bantu kuti bapite, ndipo beve banadalisa mfumuyo na kupita kwawo na chimwemwe na mitima yokondwa chifukwa cha zabwino zonse zimene Yehova anachitira Davide mutumiki wake, na Israeli, bantu bake.

Chapter 9

¹ Solomoni atatha kumanga nyumba ya Yehova, ndi nyumba ya mfumu, ndi kuchita zonse zimene anafuna kuchita, ² Yehova anaonekera kwa Solomo kachiwiri, monga anawonekera kwa iye ku Gibeoni. ³ Pamenepo Yehova anati kwa iye, Ndamva pemphero lako ndi pempho lako lopempha chifundo limene wapempha pamaso panga. moyo udzakhalapo nthawi zonse. ⁴ Koma iwe, ukadzayenda pamaso panga monga Davide atate wako anayenda ndi mtima wangwiro ndi woongoka, kumvera zonse ndinakulamulira iwe, ndi kusunga malemba anga ndi malemba anga, ⁵ pamenepo ndidzakhazikitsa mpando wachifumu wa ufumu wako pa Israele kosatha; monga ndinalonjeza Davide atate wako, ndi kuti, Pa mpando wachifumu wa Israyeli sipadzakhala mbumba yako. ⁶ Koma mukatembenuka, inu kapena ana anu, osasunga malamulo anga, ndi malemba anga amene ndakupatsani pamaso panu, ndipo mukamuka kukalambira milungu yina, ndi kuigwadira, ⁷ ndidzaononga Israyeli kuwachotsa m'dziko la Israyeli. nthaka imene ndawapatsa; ndi nyumba iyi ndapatulira dzina langa, ndidzayitaya pamaso panga; ⁸ Kachisi ameneyu adzakhala mulu wabwinja, ndipo aliyense wodutsapo adzadabwa kwambiri ndipo adzaimba mluzi. Iwo adzafunsa kuti, 'N'chifukwa chiyani Yehova wachitira zimenezi dziko ili ndi nyumba iyi?' ⁹ Enanso adzayankha kuti, 'Chifukwa chakuti anasiya Yehova Mulungu wawo, amene anatulutsa makolo awo m'dziko la Iguputo, ndipo anagwira milungu ina ndi kuigwadira ndi kuigwadira. N'chifukwa chake Yehova wawabweretsera tsoka lonseli.' ¹⁰ Ndipo kunali, pakutha zaka makumi awiri, Solomo anatsiriza kumanga nyumba ziwirizo, Kacisi wa Yehova ndi nyumba ya mfumu. ¹¹ Tsopano Hiram mfumu ya Turo anapatsa Solomo mitengo ya mkungudza ndi mikungudza, ndi golidi, zonse zimene Solomo anafuna, motero Mfumu Solomo inapatsa Hiram mizinda 20 m'dziko la Galileya. ¹² Hiram anaturuka ku Turo kukaona midzi imene Solomo anampatsa, koma sanamkomera. ¹³ Ndipo Hiram anati, Ndi midzi yotani iyi wandipatsa ine, mbale wanga? Hiram anawatcha Dziko la Kabul, limene amalitchulabe mpaka pano. ¹⁴ Hiram anatumiza kwa mfumu matalente 120 agolide. ¹⁵ Izi ndi nkhani za anthu okakamiza amene Mfumu Solomo analamula kuti amange kachisi wa Yehova ndi nyumba yake yachifumu, Milo, linga la Yerusalemu, Hazori, Megido, ndi Gezeri. ¹⁶ Farao mfumu ya Aigupto anakwera nalanda Gezeri. Anautentha ndi kupha Akanani a mumzindawo. Kenako Farao anapereka mzindawu kwa mwana wake wamkazi, mkazi wa Solomo, monga mphatso ya ukwati. ¹⁷ Choncho Solomo anamanganso Gezeri, ndi Beti-horoni wakumunsi, ¹⁸ Baalati ndi Tamara m'chipululu cha m'dziko la Yuda, ¹⁹ ndi mizinda yosungiramo zinthu zonse imene anali nayo, ndi mizinda ya magaleta ake, mizinda ya apakavalo ake, ndi chilichonse chimene anafuna kumanga. chifukwa cha kukondwera kwake m'Yerusalemu, m'Lebano, ndi m'maiko onse a ulamuliro wake. ²⁰ Anthu onse amene anatsala mwa Aamori, Ahiti, Aperizi, Ahivi, ndi Ayebusi, amene sanali a ana a Israyeli, ²¹ mbadwa zawo zotsala pambuyo pawo m'dziko, amene ana a Israyeli. Sanathe kuwaononga konse; Solomo anawagwiritsa ntchito yaukapolo, momwemo mpaka lero. ²² Koma Solomo sanagwiritse ntchito yokakamiza anthu a Isiraeli. Amenewa ndiwo anali asilikali ake, atumiki ake, akalonga ake, akapitawo ake, akuluakulu a asilikali ake a magaleta, ndi apakavalo ake. ²³ Amenewa analinso akapitawo akuluakulu oyang'anira akapitawo amene anali kuyang'anira ntchito za Solomo. ²⁴ Mwana wamkazi wa Farao anachoka mumzinda wa Davide n'kupita ku nyumba imene Solomo anam'mangira. Pambuyo pake, Solomo anamanga Milo. ²⁵ Katatu caka ciliconse Solomo anali kupeleka nsembe zopsereza ndi zacyanjano pa guwa lansembe limene anamangira Yehova, nafukiza nazo zofukiza pa guwa lansembe limene linali pamaso pa Yehova. Chotero amalaliza kachisi ndipo tsopano anali kuligwiritsa ntchito. ²⁶ Mfumu Solomo inamanga zombo zankhondo ku Ezioni Geberi, pafupi ndi Elati m'mphepete mwa Nyanja Yofiira m'dziko la Edomu. ²⁷ Hiram anatumiza atumiki ku zombo za Solomo, amalinyero odziwa bwino nyanja, pamodzi ndi antchito a Solomo. ²⁸ Iwo anapita ku Ofiri pamodzi ndi atumiki a Solomo. Kumeneko anabweretsa matalente 420 agolide kwa Mfumu Solomo.

Chapter 10

¹ Mfumu yaikazi ya ku Sheba itamva za Solomo za dzina la Yehova, inadza kudzamuyesa ndi mafunso ovuta. ² Iye anafika ku Yerusalemu ndi gulu lalitali kwambiri, ngamila zonyamula zonunkhira, golide wambiri, ndi miyala yamtengo wapatali. Atafika, anauza Solomo zonse zimene zinali mumtima mwake. ³ Solomo anayankha mafunso ake onse. Palibe chomwe adafunsa chomwe mfumu sinayankhe. ⁴ Mfumu yaikazi ya ku Sheba itaona nzeru zonse za Solomo, ndi nyumba yaufumu imene anamanga, ⁵ ndi cakudya ca patebulo pace, ndi pokhala anyamata ace, ndi nchito ya anyamata ace, ndi zobvala zao, ndi operekera chikho chake, ndi njira imene anaperekera nsembe zopsereza. zopereka m'nyumba ya Yehova, munalibenso mpweya mwa iye. ⁶ Iye anauza mfumu kuti: “Zoonadi, mbiri imene ndinaimva m'dziko langa la mawu anu ndi nzeru zanu. ⁷ Sindinakhulupirire uthengawo mpaka ndinabwera kuno, ndipo tsopano maso anga aona. Sindinauzidwe theka! Mwanzeru ndi m'chuma mwaposa mbiri imene ndinaimva. ⁸ Odala akazi anu, ndi odala atumiki anu amene amaimirira pamaso panu nthawi zonse, chifukwa amva nzeru zanu. [[Mabaibulo ena achihebri amati: “Odala amuna anu” . Matembenuzidwe akale achi Greek akuti “Odala ndi akazi anu” . Ambiri amaganiza kuti n'kutheka kuti mawu oti “akazi” anawerengedwa molakwika kuti “amuna” , chifukwa mawu awiri Achihebri amafanana kwambiri.]] ⁹ Alemekizeke Yehova Mulungu wanu, amene anakondwera nanu, amene anakuikani pa mpando wachifumu wa Israyeli. Pakuti Yehova anakonda Isiraeli mpaka kalekale, ndipo wakupangani kukhala mfumu kuti muzichita zinthu mwachilungamo ndi mwachilungamo.” ¹⁰ Anapatsa mfumu matalente 120 a golidi, ndi zonunkhira zambiri, ndi miyala ya mtengo wake; Palibe zonunkhiritsa zomwe mfumukazi ya ku Seba inapatsa Mfumu Solomo inaperekedwanso. ¹¹ Zombo za Hiram zimene zinkabwera ndi golidi wochokera ku Ofiri zinabweranso ndi mitengo ya m'bawa yambiri ndi miyala yamtengo wapatali yochokera ku Ofiri. ¹² Mfumuyo inapanga zoimiritisa zamatabwa za m'bawa za kachisi wa Yehova, + ndi za nyumba ya mfumu, ndi azeze ndi azeze za oimba. Mitengo ya mkungudza yotere sinabwere kapena kuonekanso mpaka lero. ¹³ Mfumu Solomo inapatsa mfumukazi ya ku Sheba chilichonse chimene inafuna ndi chilichonse chimene inapempha, kuwonjezera pa zimene Solomo anapatsa mfumukazi ya ku Seba. Chotero iye anabwerera kudziko la kwawo pamodzi ndi antchito ake. ¹⁴ Tsopano kulemera kwa golide amene anabwera kwa Solomo m'chaka chimodzi kunali matalente 666, ¹⁵ osawerengera golide amene amalonda ndi amalonda ankabwera nawo. Mafumu onse a Arabiya ndi abwanamkubwa a m'dzikolo anabweretsanso golide ndi siliva kwa Solomo. ¹⁶ Mfumu Solomo inapanga zishango zazikulu mazana awiri zagolide wosakaniza ndi zitsulo zina. Masekeli mazana asanu ndi limodzi a golidi analowa m'modzi. ¹⁷ Anapanganso zishango mazana atatu zagolide wosakaniza ndi zitsulo zina. chishango chilichonse chinali ndi mamina atatu agolidi; mfumu inawaika m'nyumba ya mfumu ya Nkhalango ya Lebanoni. ¹⁸ Kenako mfumu inapanga mpando waukulu wa minyanga ya njovu n'kuukuta ndi golide woyengeka bwino. ¹⁹ Panali masitepe 6 opita kumpando wachifumuwo, ndipo nsonga yake inali yozungulira kumbuyo kwake. Kumbali zonse za mpandowo kunali zoikiramo manja, ndi mikango iwiri itaimirira m'mbali mwa mawondowo. ²⁰ Mikango khumi ndi iwiri inayimirira pamakwerero, imodzi mbali iyi ndi imodzi ya makwerero asanu ndi limodzi. Panalibe mpando wachifumu wonga umenewo mu ufumu wina uliwonse. ²¹ Zikho zonse zomweramo Mfumu Solomo zinali zagolide, ndi zikho zonse zomweramo za m'Nkhalango ya Lebanoni zinali zagolide woyenga bwino. Panalibe siliva, chifukwa siliva sanali wofunika m'masiku a Solomo. ²² Mfumuyo inali ndi zombo za ku Tarisi panyanja pamodzi ndi gulu la Hiram. Zombozo zinkabwera ndi golidi, siliva, minyanga ya njovu kamodzi pa zaka zitatu zilizonse, anyani ndi anyani. ²³ Choncho Mfumu Solomo inaposa mafumu onse a padziko lapansi pa chuma ndi nzeru. ²⁴ Anthu onse a padziko lapansi anafuna pamaso pa Solomo kuti amve nzeru zake zimene Mulungu anaika mumtima mwake. ²⁵ Amene anabwera kudwabwera ndi msonkho, + zotengera zasiliva, zagolide, zovala, zida zankhondo, zonunkhira, akavalo ndi nyuru chaka ndi chaka. ²⁶ Solomoni anasonkhanitsa magaleta ndi apakavalo. Anali ndi magareta 1,400 ndi apakavalo 12,000 amene anawaika m'mizinda ya magaleta ndiponso ku Yerusalemu. ²⁷ Mfumuyo inali ndi siliva ku Yerusalemu ngati miyala yapansi. Anachulukitsa mitengo ya mkungudza + ngati mikuyu ya m'zigwa. ²⁸ Akavalo amene anali a Solomo anagula ku Iguputo, + ndipo Kuwe ndi amalonda a mfumu anali kuwagula ku Kuwe. ²⁹ Magareta anakwera kucokera ku Aigupto pa mtengo wa masekeli mazana asanu ndi limodzi a siliva, ndi akavalo masekeli 150. Ambiri a iwo anagulitsidwa kwa mafumu onse a Ahiti ndi Aaramu.

Chapter 11

¹ Tsopano Mfumu Solomo inakonda akazi ambiri achilendo, kuphatikizapo mwana wamkazi wa Farao, akazi achimowabu, Aamoni, Aedomu, Asidoni, ndi Ahiti. ² Anali a mitundu imene Yehova anauza ana a Isiraeli kuti: “Musapite pakati pawo kukakwatira kapena kukwatiwa, kapena kuti iwowo asalowe pakati panu, chifukwa adzatembenuzira mitima yanu kwa milungu yawo. Mosasamala kanthu za lamulo limeneli, Solomo anakonda akazi ameneŵa mwachikondi. ³ Solomoni anali ndi akazi mazana asanu ndi awiri, ana aakazi, ndi adzakazi mazana atatu. Akazi ake anapatutsa mtima wake. ⁴ Pakuti pamene Solomo anakalamba, akazi ake anapambutsa mtima wake atsate milungu yina; mtima wake sunadzipereka kwathunthu kwa Yehova Mulungu wake, monga mtima wa Davide atate wake. ⁵ Pakuti Solomo anatsatira Asitoreti mulungu wamkazi wa Asidoni, ndi kutsatira Moleki fano lonyansa la Aamoni. ⁶ Solomoni anachita choipa pamaso pa Yehova; sanatsata Yehova ndi mtima wonse monga anachitira Davide atate wake. ⁷ Pamenepo Solomoni anamangira Kemosi fano lonyansa la Mowabu malo okwezeka paphiri la kum'mawa kwa Yerusalemu, ndiponso anamangira Moleki fano lonyansa la ana a Amoni. ⁸ Anamangiranso akazi ake onse achilendo malo okwezeka, amene ankafukizapo nsembe zautsi ndi kupereka nsembe kwa milungu yawo. ⁹ Yehova anakwiyira Solomo chifukwa mtima wake unapatuka kwa iye, Mulungu wa Isiraeli, ngakhale kuti anaonekera kwa iye kawiri, ¹⁰ ndipo anamulamula kuti asatsatire milungu ina. Koma Solomo sanamvere zimene Yehova anamuza. ¹¹ Choncho Yehova anauza Solomo kuti: “Popeza wachita zimenezi, osasunga pangano ndi malemba anga amene ndinakulamulira, ndithu ndidzang'amba ufumuwo kuuchotsa kwa iwe ndi kuupereka kwa mtumiki wako, ¹² koma chifukwa cha Davide atate wako. Sindidzachita zimenezi udakali ndi moyo, koma ndidzaukhadzula m'manja mwa mwana wako, ¹³ koma ndidzaupereka kwa mwana wako fuko limodzi chifukwa cha Davide mtumiki wanga wa Yerusalemu, umene ndausankha.” ¹⁴ Pamenepo Yehova anamuutsira Solomo mdani, ndiye Hadadi Medomu. Iye anali wa banja lachifumu la Edomu. ¹⁵ Pamene Davide anali ku Edomu, Yowabu kazembe wankhondo anapita kukaika akufa, onse amene anaphedwa mu Edomu. ¹⁶ Yowabu ndi Aisrayeli onse anakhala kumeneko miyezi isanu ndi umodzi mpaka anapha amuna onse a ku Edomu. ¹⁷ Koma Hadadi anathawira ku Aigupto pamodzi ndi Aedomu ena, anyamata a atate wake, Hadadi akali mwana. ¹⁸ Iwo anachoka ku Midyani n'kukafika ku Parana, kumene anatenga amuna n'kupita nawo ku Iguputo kwa Farao mfumu ya Iguputo, amene anam'patsa nyumba ndi malo ndi chakudya. ¹⁹ Farao anamkomera mtima kwambiri Hadadi, moti Farao anampatsa mkazi, mlongo wake wa mkazi wake, mlongo wake wa Tapenesi mfumukazi.

Chapter 13

¹ Munthu wa Mulungu anachokela ku Yuda na mau ya Yehova anabwela ku Beteli. Yerobowamu anaimilila pafupi na guwa yansembe kuti ashoke lubani. ² eve analilila pa guwa yansembe mu mau a Yehova kuti: "Guwa yansembe, guwa yansembe! Ivi nde vama Yehova anakamba, 'Ona, mwana mwamuna zina yake Yosiya azabadwa m'banja ya Davide, ndipo azapeleka nsembe kuli iwe nsembe ya misanje yamene azashokela lubani kuli iwe; pali iwe aza shoka ma bonzo ya ba banthu. ³ Ndipo munthu wa Mulungu anapasa chilangizo siku yamene ija, kukamba, Ichi nichilangizo kuti Yehova akamba: Onani, guwa ya nsembe yagabanikana; ndipo milota yasanduliwa.'" ⁴ Pamene mfumu ananvela vamene mwana mwamuna wa Mulungu anakamba, kuti analilila guwa yansembe ku Beteli, Yeroboamu anatambulula kwanja yake kuchokela pa guwa, kukamba, "Mgwileni." kwanja yamene anatambulula mwamuna inayuma, kuti asabwewelele kuli eve. ⁵ (Guwa yansembe inagabanikana ndipo milota inasanulidwa paguwa, monga kunalongosolela na chilangizo chamene munthu wa Mulungu uja anapleleka mu mau ya Yahweh.) ⁶ Mfumu Yerobiamu anayanka nakukamba kuli munthu wa Mulungu ati, "Pempa kuti Yehova Mulungu wako ankale nau bwino ndipo unipempelele, kuti kwanja yanga ibwelele kuli ine." Kapolo wa Mulungu anapempela kuli Yehova, ndipo kwanja ya mfumu inabwezewa kuli eve, ndipo chinankala monga poyamba. ⁷ Mfumu inauza kapolo wa Mulungu uja, "bwela kunyumba naine ukapumule, ndipo nizakupasa mphaso." ⁸ Kapolo wa Mulungu ana kamba kuli mfumu, "nangu unipase pakati pa chuma chako, sinizayenda naiwe, kapena kudya kapena kumwa manzi pamalo pano, ⁹ chifukwa Yehova ananilamulila mu mau yake kuti, 'Usadye mukate kapena kumwa manzi, kapena kubwelela panjila yamene wabwelele.'" ¹⁰ kapolo wa Mulungu leka njila ina ndipo sanabwelele kunyumba kwake kupitila njila yamene anapitila ku Beteli. ¹¹ Manje panali mneneli mukulu wamene anakala ku Beteli, ndipo umozi mwana wake paba muna anabwela kumu uza vonse vamene kapolo wa Mulungu anachita pa siku ija mu Beteli. bana bake bamuna banamu uza mau yamene kapolo wa Mulungu anakamba kuli mfumu. ¹² Ba tate babo banakamba kuli beve, "Anayenda njila iti?" Manje bana bake ba muna banaona njila ya kapolo wa Mulungu yochokela ku Yuda. ¹³ Ndipo anakamba kuli bana bake bamuna, Nimangileni mbela pa bulu wake. Ndipo anamangilila bulu, naku; ikwela. ¹⁴ Mneneli mukulu pa sogolo pa kapolo wa Mulungu anamupeza ankala pansa pa mtengo ikulu; ndipo anakamba kuli eve, Ndiwe kapoo wa Mulungu anachokela ku Yuda? Eve anayanka, "Ndine." ¹⁵ Ndipo mneneli mukulu anakamba kuli eve, "Bwelela naine kunyumba ukadye na chakudya." ¹⁶ kapolo wa Mulungu anayanka kuti, "Sindingabwelele naiwe kapena kungena naiwe, kapena kudya chakudya kapena kumwa manzi pamozi naiwe pamalo yano, ¹⁷ chifukwa aninilamulila Yehova kuti, 'Usadye chakudya kapena kumwa manzi kwamene uko, ndipo musabwelele njila yamene munabwelele.'" ¹⁸ Ndipo mneneli mukulu anakamba kuli eve, naine ndine mneneli monga iwe, ndipo mngeli anakamba kuli ine mu mau ya Yehova, kukamba, Mubwele naye kunyumba kwako kuti akadye chakudya na kumwa manzi. "Koma anali kunama kuli kapolo wa Mulungu. ¹⁹ koma kapolo wa Mulungu anabwelele na mneneli mukulu ndipo anakadya chakudya munyumba mwake na kumwa manzi. ²⁰ Pamene banankala pa tebo, mau ya Yehova yanabwela kuli mneneli wamene anamuleta kuli eve, ²¹ ndipo ana lila kuli kapolo wa Mulungu wamene anabwela kuchokela ku Yuda, kukamba, Yehova akamba, Chifukwa sunamvela mau ya Yehova ndipo simunasunge lamulo yamene Yehova Mulungu wanu anakupasani, ²² koma munabwela na kudya na kumwa manzi kumalo kwamene Yehova anaku uzani kuti musadye kapena kumwa manzi, tupi yanu sizashikiwa m'manda yaba tate bano. ²³ Kuchokela kudya na kumwa, mneneli anakwela bulu kapolo wa Mulungu, muntu wamene anabwelele naye. ²⁴ Pamene kapolo wa Mulungu anayenda, nkalamu ina mukumana panjila nakumupaya, ndipo tupi yake inasala panjila. Bulu inaimilia pambali pake, ndipo nkalamu nayeve inaimilia pafupi pa tupi. ²⁵ pamene bamuna bana pita naku ona tupi ina sala panjila, ndipo nkalamu inamilila pafupi na tupi, banabwela naku kamba mu mzinda mwamene mneneli mukulu enzokala. ²⁶ Pamene mneneli wamene anamubwealesa kuchokela ku njila ija anakamba, "Ni kapolo wa Mulungu wamene sananvele mau ya Yehova. Chifukwa ichi Yehova anamupeleka kuli nkalamu, ndipo ana mujubajuba mutungono naku mu paya, mau ya Yehova anamuchenjeza. " ²⁷ Ndipo mneneli mukulu anakamba na bana bake bamuna, kukamba, "Mangililani bulu yanga," ndipo banaimangilila. ²⁸ Anayenda nakapeza tupi inasala panjila, bulu na nkalamu kuimilila pafupi na tupi. Nkalamu sinadye chitumbi kapena ku gonjesa bulu. ²⁹ Pamene mneneli ananyamula chitumbi cha kopolo wa Mulungu, ana chiika pa bulu, naku chibweza. anabwela mzinda kwao kumulila na kumushika m'manda. ³⁰ Anayika chitumbi chake m'manda wake, ndipo banamulia, kuti, "soka, m'bale wanga!" ³¹ Pamene ana mushika m'manda, mneneli mukulu anakamba anakamba kuli bana bake ba muna, kuti, "Ngati nafa mukanishike m'manda mwamene kapolo wa Mulungu anashikiwa. Ikani mabonzo yanga pafupi nama bonzo yake. ³² Koma uthenga ana kambilila mu mau ya Yehova, kunyamukila guwa ya nsembe mu Beteli, na manyumba yonse yakumalo yokwezeka m'mizinda ya Samariya, viza chitika zoona." ³³ kuchoka ichi Yerobiamu sanasiye

kuchoka ku njila zake zoipa, koma anapitiliza kusanka bansembe bosayenla kuchokela ku bantu osiyanasiyana. Aliyense wamene anatumikila anali kupatula bansembe. ³⁴ Iyi nkhani inankala chimo ku banja ya Yeroboamu ndipo inachitisa kuti banja yake iwonongeke na kufafaniziwa pa ziko yapansi.

Chapter 14

¹ Pa nthawiyo Abiya mwana wa Yerobiamu anadwala kwambiri. ² Yerobiamu anati kwa mkazi wake, Nyamukatu, udzizimbale, kuti usadziwike kuti ndi mkazi wanga, nupite ku Silo, popeza Ahiya mneneri ali komweko; ndiye amene ananena za ine, kuti ndidzakhala mfumu. ³ Utenge mitanda ya mikate khumi, mikate ndi mtsuko wa uchi ndipo upite kwa Ahiya. ⁴ Mkazi wa Yerobiamu anachita chomwecho; Kenako ananyamuka n'kupita ku Silo n'kukafika kunyumba ya Ahiya. Koma Ahiya sanatha kuona; anasiya kuona chifukwa cha ukalamba. ⁵ Yehova anati kwa Ahiya, Taona, mkazi wa Yerobiamu akudza kudzafunsira kwa iwe za mwana wake; . ⁶ Ahiya atamva kugunda kwa mapazi ake akulowa pakhomo, anati: "Lowa, mkazi wa Yerobiamu. N'chifukwa chiyani ukudziyerekezera kuti ndiwe munthu?" ⁷ Ukauze Yerobiamu kuti, 'Yehova Mulungu wa Isiraeli wanena kuti, 'Ndinakukweza pakati pa anthu kuti ndikuike kukhala mtsogoleri wa anthu anga Aisiraeli, ⁸ ndipo ndinang'amba ufumuwo kuuchotsa pa banja la Davide ndi kuupereka kwa iwe monga Davide mtumiki wanga, amene anasunga malamulo anga, nanditsata ine ndi mtima wake wonse, kuchita yekha zoyenera pamaso panga. ⁹ M'malo mwake, wachita zoipa kwambiri kuposa onse amene anakhalapo iwe usanakhale. Wapanga milungu yina, ndi kupanga mafano osungunula kuti undikwiyitse, ndipo unandikankha kumbuyo kwako. ¹⁰ Cifukwa cace taonani, ndidzatengera nyumba ya Yerobiamu coipa; Ndidzapha ana onse aamuna mu Isiraeli, kaya akhale kapolo kapena mfulu, ndipo ndidzachotsa nyumba ya Yerobiamu ngati munthu wotenthetsetsa ndowe mpaka kutha. ¹¹ Aliyense wa Yerobiamu amene adzafera mumzindawo, agalu adzamudya, ndipo aliyense wofera kutchire adzamudya ndi mbalame za m'mlengalenga, pakuti ine Yehova ndanena zimenezi. ¹² Chotero nyamuka, mkazi wa Yerobiamu, bwerera kunyumba kwako; mapazi ako akalowa m'mudzi, mwana Abiya adzafa. ¹³ Aisiraeli onse adzamalira ndi kumuika m'manda. Ndi iye yekha wa m'banja la Yerobiamu amene adzalowa m'manda, chifukwa mwa iye yekha, m'nyumba ya Yerobiamu, munapezeka chilichonse chokoma pamaso pa Yehova Mulungu wa Isiraeli. ¹⁴ Komanso Yehova adzautsa mfumu ya Isiraeli imene idzaphe banja la Yerobiamu pa tsiku limenelo. Lero ndi tsiku limenelo, pompano. ¹⁵ Pakuti Yehova adzaukira Isiraeli ngati bango likugwedezeke m'madzi, ndipo adzazula Isiraeli m'dziko labwinoli limene anapereka kwa makolo awo. Iye adzawamwaza kutsidya lina la Mtsinje wa Firate, chifukwa iwo anadzipangira mizati ya Asera ndi kuputa mkwiyo wa Yehova. ¹⁶ Iye adzasiya Isiraeli chifukwa cha machimo a Yerobowamu, machimo amene anachita, ndiponso amene anachimwitsa nawo Isiraeli."

¹⁷ Pamenepo mkazi wa Yerobiamu ananyamuka, nachoka, nafika ku Tiriza. Pamene anafika pakhomo la nyumba yake, mwanayo anamwalira. ¹⁸ Aisiraeli onse anamuika m'manda n'kumulira monga mmene Yehova ananenera kudzera mwa mtumiki wake Ahiya mneneri. ¹⁹ Nkhani zina zokhudza Yerobiamu, mmene anamenyera nkondo+ ndi mmene analamulirira, zinalembedwa m'buku la zochitika za mafumu a Isiraeli. ²⁰ Yerobiamu analamulira zaka 22, ndipo anagona pamodzi ndi makolo ake, ndipo Nadabu mwana wake anayamba kulamulira m'malo mwake. ²¹ Tsopano Rehobowamu mwana wa Solomo anali kulamulira ku Yuda. Rehobowamu anali wa zaka 41 pamene anayamba kulamulira, ndipo analamulira zaka 17 ku Yerusalemu, mzinda umene Yehova anausankha mwa mafuko onse a Isiraeli kuti aikemo dzina lake. Dzina la amayi ake linali Naama Mamoni. ²² Yuda anacita coipa pamaso pa Yehova; anamcititsa nsanje ndi zocimwa zao, zopambana zonse anazicita makolo ao. ²³ Iwo anadzimangiranso malo okwezeka, zipilala zamiyala ndi mizati ya Asera pa zitunda zonse zazitali ndi pansi pa mtengo uliwonse wa masamba obiriwira. ²⁴ M'dzikomo munalinso mahule achipembedzo. Anachita zonyansa ngati zimene amitundu amene Yehova anawaingitsa pamaso pa ana a Isiraeli. ²⁵ Ndiyeno m'chaka chachisanu cha Mfumu Rehobowamu, Sisaki mfumu ya ku Iguputo inabwera kudzamenyana ndi Yerusalemu. ²⁶ Iye anatenga chuma cha m'nyumba ya Yehova ndi chuma cha m'nyumba ya mfumu. Iye anachotsa chirichonse; anatenganso zishango zonse zagolide zimene Solomo anapanga. ²⁷ Mfumu Rehobowamu inapanga zishango zamkuwa m'malo mwake, n'kuzipereka m'manja mwa akuluakulu a asilikali olondera zitseko za nyumba ya mfumu. ²⁸ Ndipo kunali kuti, polowa mfumu m'nyumba ya Yehova, odikira ananyamula; Kenako anali kuwabweretsa kunyumba ya alonda. ²⁹ Nkhani zina zokhudza Rehobowamu ndi zonse zimene anachita, zinalembedwa m'buku la zochitika za m'masiku a mafumu a Yuda. ³⁰ Panali nkondo yokhazikika pakati pa Rehobowamu ndi Yerobiamu. ³¹ Choncho Rehobowamu anagona pamodzi ndi makolo ake ndipo anaikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake mu Mzinda wa Davide. Dzina la amayi ake linali Naama Mamoni. Abiya mwana wake anakhala mfumu m'malo mwake.

Chapter 20

¹ Beni-Hadadi mfumu ya Aramu anaunjika bankondo bake bonse pamozi. Panali naye mafumu yangono yangono yali 32, na makavalo na magareta. Anayenda pamwamba, kuzunguluka samaliya na kumenyana nayo ². Anatuma ntumi mu muzinda kuli Ahabu mfumu ya Israeli, nakukamba kuli eve, "Ben Hadadi akamba ivi: ³ 'Siliva yako na golide yako ni yanga. Kuikilapo futi bakazi bako na bana, babwino maningi, manje ni banga.' " ⁴ Mfumu ya Israeli inayanka nakukamba ati, "Chili Monga mwamene wakambila, mbuye wanga mfumu. Ine na vonse vamene nilinavo ni vako." ⁵ ntumi zinabwela futi na kukamba ati, "Ben Hadadi akamba ivi, 'Ninakutumizila mau wokamba kuti unipase siliva yako, golide yako, bakazi bako, na bana bako. ⁶ Koma nizatuma bantchito banga kuli iwe mailo ntau yamene iyi, ndipo bazasakila sakila munyumba yako na mumanyumba yabanchito bako. Bazagwila na manja yao, nakuchosapo vonse vamene visangalasa menso yako.' " ⁷ Pamene apo mfumu ya Israeli inayitana bakulu bonse ba muziko ija nakukamba ati, "Napapata zibani na kuwona mwamene muntu uyu afunila mavuto. Atumiza utenga kuli ine kuti atenge bakazi banga, bana, siliva na golide, ndipo ine sininamu kanile." ⁸ Bakulu bonse na bantu bonse bana kamba kuli Ahabu "Musamumvele kapena kuchita vamene afuna." ⁹ Pamenepo Ahabu anauza bautenga ba Beni-hadadi kuti, "Uzani mbuye wanga mfumu kuti, 'Nivomeleza pavonse kuti munatumiza kapolo wanu kuchita paulendo woyamba, koma sinizavomela futi.' " ndipo ntumi zinachoka nakupeleka yanko kuli Ben Hadadi. ¹⁰ Ndipo Ben Hadadi anatumiza yanko yake kuli Ahabu, nakukamba ati, "Milungu zinichite so chabe nakuchilapo, " ngati milota ya mu samalia ingakwanile bantu bonse bamene banikonka kutengako che mukwanja," ¹¹ Mfumu ya Israeli inayanka nakukamba ati, "Uza Beni-Hadadi kuti, 'Palibe wamene avala zida zake ayenela kuzimvela monga azaivula.' " ¹² Ben Hadadi anamvela utenga uwu pamene anali kumwa, eve na mfumu zinali pansi pake zamene zinali mumahema zawo. Ben Hadadi analamula banchito bake kuti, "Konzekelani nkondo." pamene apo banakonzekela mumalo ya nkondo kuti bamenyane na muzinda na muzinda. ¹³ Ndipo onani, muneneli anabwela kuli Ahabu mfumu ya Israyeli, nakukamba ati, Yehova akamba, ' wayiona gulu yankondo ikulu iyi? Ona, nizayiika mumanja mwako lelo, ndipo uzaziba kuti ndine Yehova. , ¹⁴ "Ahabu anayanka kuti, pali ndani?" Yehova anayanka nakukamba ati, "Pali banyamata bosebenezela bakazembe bamalo." Ndipo Ahabu anakamba ati, "Nindani wamene azayamba kumenya nkondo iyi?" Ndipo Yehova anayanka, "Iwe." ¹⁵ pamene apo Ahabu anasonkanisa banyamata bamene banalli kusebenzela bakazembe ba mumalo. Banali 232. Kuchoka apo anasonkanisa basilikali bonse, gulu yonse yankondo ya Israyeli; yokwanila 7000. ¹⁶ Banayenda mu zuba. Ben Hadadi enze kumwa moba mutenti yake mpaka kukolewelatu, eve pamozi na mafumu yangonoyangono 32 yamene yenze kumutandiza. ¹⁷ Bankondo bafana bamene benzo tumikila bakazembe ba mumalo banayenda pasogolo. Ndipo Ben Hadadi anauziwa na bazondi bamene enze anatuma , "Bamuna bachokela ku Samariya." ¹⁸ Ben Hadadi anakamba, "Kaya ngati babwelela mutendele olo nkondo nkondo, baleteni bamoyo." ¹⁹ Mwaicho banyamata benzo tumikila bakazembe ba madela banayenda kuchoka mu muzinda ndipo gulu yabankondo inabakonka. ²⁰ Aliyense anapaya muzake. Baku Aaramu banataba ndipo Israyeli anaba konka pambuyo. Beni-Hadadi mfumu yaku Aramu anataba pakavalo pamozi na bamuna boyendesa makavalo. ²¹ kuchoka apo mfumu ya Israyeli inayenda kumenya makavalo na magaleta yao, na kupaya baku Aramu bambili maningi. ²² Manje muneneli anabwela kuli mfumu ya Isilayeli nakukamba kuli yeve," Yenda, ukazilimbise, na kumvesesa na kukonza vameme uchita, chifukwa pakusila kwa chaka mfumu ya Aramu izabwela kumenyana naiwe futi. ²³ Banchito ba mfumu ya Aramu banakamba kuli eve, "Mulungu wabo ni Mulungu wa mapili. Ndiye chifukwa chake benze nampamvu kuchila ise. Koma manje tiyeni timenyane nabo muchigwa, ndipo tizankala bolimba kubachila. ²⁴ Mwaicho muchite ivi: Chosani mamfumu yonse pamalo yao yaulamulilo wao nakufakapo bakulu bakulu bankondo. ²⁵ Nyamulani gulu yankondo monga yamene munataya — kavalo mumalo mwa kavalo na galeta mumalo ya galeta- kuti tingamenyane nabo muchigwa. Pamene apo mosakaikila tizankala na mpamvu kubachila . Mwaicho Ben Hadadi anamvela vamene banamuuza na kuchita vamene banamulangiza. ²⁶ Pambuyo poyamba chaka chamanje, Ben Hadadi anasonkanisa ma Aaramu na kuyenda ku Afeki kumenyana na Isirayeli. ²⁷ Bantu baku isilayeli banasonkanisiwa na kupasiwa kuti bamenyane nabo. Bantu baku isilayeli banamanga misasa pasogolo pabo monga tumagulu tubili twa mbuzi, koma ma Aaramu banazula malo yonse. ²⁸ Pamene apo muntu wa Mulungu anabwela pafupi na kukamba na mfumu ya Isirayeli ati, " Yehova akamba: 'Chifukwa ba Aaramu bakamba kuti Yehova ndiye mulungu wa kumapili, koma si Mulungu wa vigwa, nizaika iyi gulu yambili ya nkondo mukwanja yako ndipo uzaziba kuti ndine Yehova.' " ²⁹ Mwaicho magulu yankondo yanasonkana moyanganana pa masiku 7. Manje pasiku yasabata nkondo inayamba. Bantu baku isilayeli banapaya basilikali baku Aaramu 100,000 pasiku imozi. ³⁰ Banasala banatabila ku Afeki, mumuzinda, ndipo chipupa chinagwela pali bamuna 27,000 bamene banasala. Ben Hadadi anataba nakuyenda mu muzinda, muchipinda chamukati. ³¹ Bancito ba Ben Hadadi banakamba kuli eve, "Ona manje, tamvela kuti

mfumu za nyumba ya Isirayeli ni mfumu zachifundo. Napapata tiyeni timange vovala vamasaka muchiuno mwatu na ntambo kumitu zatu, na kuyenda kuli mfumu yaku Isirayeli. Mwamwai azapulumuswa umoyo wako. " ³² Mwaicho banavala vovala vamasaka muchiuno na ntambo mumitu zao na kuyenda kuli mfumu ya Isirayeli nakukamba ati, "wanchito wanu Ben Hadadi anakamba, 'Napapata lekani ninkale wa moyo.'" Ahabu anakamba, "akali wa moyo? ni mubale wanga. " ³³ Manje bamuna banali kumvelela chizindikilo chilichonse chochokela kuli Ahabu, pameneapo mwamusanga banamuyanka kuti, "Ehe, mubale wako Ben Hadadi ali moyo." Mwaicho Ahabu anakamba, " yenda ukamulete." ³⁴ Ndipo Ben-Hadadi anakamba kuli Ahabu, "Nikubwezelani mizinda zamene batate banga banapoka batate banu, ndipo mungazipangile pogulisila mu Damasiko, mwamene batate banga banachitila ku Samariya." Ahabu anayanka, "Nizakuleka uyende na pangano iyi." ndipo Ahabu anachita naeve pangano, nakumuleka ayende. ³⁵ Muntu winango, umozi pali bana ba baneneli, anakamba kuli munzake kupitila mu mau ya Yehova, "Napapata nimenye." Koma mwamuna anakana kumumenya. ³⁶ Mwaicho muneneli anakamba kuli muneneli munzake, "Chifukwa sunamvele mawu ya Yehova, pamene apo ukanisiya, nkalamu izakupaya." Pamene apo mwamuna anayenda, nkalamu inabwela pali eve na kumupaya. ³⁷ Kuchoka apo muneneli anapeza muntu winango nakukamba, "Napapata nimenye." ndipo mwamuna uyo anamumenya na kumupanga chilonda. ³⁸ Ndipo muneneli anayenda nakuyembekeza mfumu panjila; anali anazibis na nsalu pamenso yake. ³⁹ Pamene mfumu inapitilapo, muneneli analila kuli mfumu nakukamba ati, "Wantchito wako anayenda mukutenta kwa nkondo, ndipo musilikali winanangu ana imilila nakuleta muntu kuli ine na kukamba, 'onani muntu uyu. Ngati mu njila iliyonse asoba, moyo wako uzapasiwa mumalo mwa moyo wake, olo uzafunika kulipila ndalama imozi ya siliva. ' ⁴⁰ Koma chifukwa wanchito wako enze kungo yenda yenda uku na uku, muntu anataba. " ndipo mfumu ya Israeli inamuwaza kuti, "Ichi ndiye chizankala chilango chako- iwe mwine wake wasanka." ⁴¹ Pamene apo muneneli mwamusanga musanga anachosa chomangilila mumenso mwake, ndipo mfumu ya Israeli inazindikila kuti eve enze umozi wa baneneli. ⁴² Ndipo muneneli anakamba kuli mfumu, Yehova akamba, "Pakuti walekelela muntu wamene nenze nina peleka kuchionongoke, moyo wako uzankala mumalo mwa moyo wake, na bantu mumalo mwa bantu bake. ⁴³ mwaicho Mfumu ya Israeli inayenda kunyumba kwake yokolewa na namkwiyo, nakufika ku Samaliya.

Chapter 21

¹ Patapita nthawi, Naboti wa ku Yezreeli anali ndi munda wa mpesa ku Yezereeli, pafupi ndi nyumba yachifumu ya Ahabu mfumu ya Samariya. ² Ahabu anauza Naboti kuti: “Ndipatse munda wako wa mpesawu kuti ukhale munda wamphesa, chifukwa uli pafupi ndi nyumba yanga. mtengo wake mumtengo.” ³ Naboti anayankha Ahabu kuti, “Yehova asandiletse kuti ndikupatseni cholowa cha makolo anga. ⁴ Choncho Ahabu analowa m’nyumba yake ali wokwiya komanso wokwiya chifukwa cha yankho limene Naboti wa ku Yezreeli anamuyankha kuti: “Sindidzakupatsa cholowa cha makolo anga.” Anagona pabedi lake, natembenuza nkhope yake, ndipo anakana kudya chakudya chilichonse. ⁵ Yezebeli mkazi wake anadza kwa iye nati kwa iye, Mtima wako uli wachisoni bwanji, osadya chakudya? ⁶ Iye anayankha kuti, “Ndinalankhula ndi Naboti wa ku Yezreeli kuti, ‘Ndipatse munda wako wa mpesa ndi ndalama zanga, kapena ngati ukufuna, ndikupatse munda wina wa mpesa umene ukhale wako. ⁷ Pamenepo iye anandiyankha kuti, ‘Sindikupatsani munda wanga wa mpesa.’” Yezebeli mkazi wake anamuyankha kuti: “Kodi sunayambenso kulamulira mu ufumu wa Isiraeli? iwe munda wa mpesa wa Naboti wa ku Yezreeli.” ^{8 10} Choncho Yezebeli analemba makalata m’dzina la Ahabu, nawadinda ndi chidindo chake, n’kuwatumiza kwa akulu ndi kwa olemkezekaka amene anakhala naye m’misonkhano, amene anali kukhala pafupi ndi Naboti. ⁹ Iye analemba m’makalatawo kuti: “Lalikirani kusala kudya ndipo mukhazikitse Naboti pamwamba pa anthuwo. Mutengerenso amuna awiri opanda pake kuti am’chitire umboni kuti, ‘Iwe watemberera Mulungu ndi mfumu.’” Kenako mum’tulutseni ndi kumuponya miyala kuti afe. ¹¹ Choncho amuna a mumzinda wa Naboti, akulu ndi anthu olemkezekaka amene anali kukhala mumzinda wa Naboti, anachita monga mmene Yezebeli anawafotokozera, monga mmene zinalembedwera m’makalata amene anawatumizira. ¹² Iwo analengeza kuti kusala kudya n’kukhazika Naboti pamwamba pa anthu. ¹³ Anthu awiri achinyengowo analowa ndi kukhala pamaso pa Naboti; ndipo anamchitira umboni Naboti pamaso pa anthu, kuti, Naboti watemberera Mulungu ndi mfumu. Kenako anamutengera kunja kwa mzinda ndi kumuponya miyala. ¹⁴ Kenako akuluwo anatumiza uthenga kwa Yezebeli kuti: “Naboti waponyedwa miyala ndipo wafa. ¹⁵ Choncho Yezebeli atamva kuti Naboti waponyedwa miyala ndi kufa, anauza Ahabu kuti: “Nyamukani, tenga munda wa mpesa wa Naboti wa ku Yezreeli, umene anakana kukupatsani ndi ndalama, chifukwa Naboti sali ndi moyo koma wafa. ” ¹⁶ Ahabu atamva kuti Naboti wafa, ananyamuka kupita kumunda wa mpesa wa Naboti wa ku Yezreeli kuti akautenge. ¹⁷ Kenako mawu a Yehova anafika kwa Eliya wa ku Tisibe, kuti: ¹⁸ “Nyamuka, pita ukakumane ndi Ahabu mfumu ya Isiraeli, amene amakhala ku Samariya, m’munda wa mpesa wa Naboti, kumene wapita kuti akautenge. ¹⁹ Ukamuuze kuti Yehova akuti, ‘Kodi wapha ndi kulanda? Pamenepo udzamuuzwa kuti Yehova akuti, ‘Pamalo pamene agalu ananyambita magari a Naboti, agalu adzanyambita magari ako, inde magari ako.’” ²⁰ Ahabu anauza Eliya kuti: “Kodi wandipeza mdani wanga? Eliya anayankha kuti: “Ndakupeza, chifukwa wadzigulitsa kuti uchite zoipa pamaso pa Yehova. ²¹ Yehova atero kwa iwe, Taona, ndidzakutengera tsoka, ndi kutha ndi kupha Ahabu ana aamuna onse, ndi kapolo, ndi mfulu m’Israyeli; ²² Ndidzayesa banja lako ngati banja la Yerobiamu mwana wa Nebati, ndi banja la Basa mwana wa Ahiya, popeza wandikwiyitsa ine, ndi kucimwitsa Israyeli. ²³ Yehova ananenanso za Yezebeli, kuti, Agalu adzadya Yezebeli pafupi ndi linga la Yezreeli. ²⁴ Aliyense wa Ahabu akafera mumzinda, agalu adzamudya. ndipo mbalame za mumlengalenga zidzadya aliyense wakufa kuthengo. ²⁵ Panalibe munthu wonga Ahabu amene anadzigulitsa kuti achite zoipa pamaso pa Yehova, amene Yezebeli mkazi wake anamuchimwitsa. ²⁶ Ahabu ananyansidwa ndi mafano, monga mwa zonse anacita Aamori, amene Yehova anawacotsa pamaso pa ana a Israyeli. ²⁷ Ahabu atamva mawu amenewa, anang’amba zovala zake n’kuvala chiguduli n’kusala kudya, n’kugona chiguduli ndi kumva chisoni kwambiri. ²⁸ Pamenepo mawu a Yehova anafika kwa Eliya wa ku Tisibe, kuti: ²⁹ “Kodi waona mmene Ahabu wadzichepetsera pamaso panga? Popeza wadzichepetsa pamaso panga, sindidzabweretsa tsoka limene likubwera m’masiku ake, + chifukwa m’tsiku la mwana wake ndidzabweretsa tsoka pa banja lake.

Chapter 22

¹ Panapita zaka zitatu popanda nkondo pakati pa Aramu ndi Aisiraeli. ² Ndiyeno m'chaka chachitatu, Yehosafati mfumu ya Yuda anatsikira kwa mfumu ya Isiraeli. ³ Ndipo mfumu ya Isiraeli inati kwa anyamata ace, Kodi mudziwa kuti Ramoti-giliyadi ndi wathu, koma siticita kanthu kuulanda m'dzanja la mfumu ya Aramu? ⁴ Ndipo anati kwa Yehosafati, Kodi udzapita nane kunkhondo ku Ramoti Gileadi? Yehosafati anayankha mfumu ya Isiraeli kuti, "Ine ndili ngati inu, anthu anga ali ngati anthu anu, ndipo akavalo anga ali ngati akavalo anu." ⁵ Yehosafati anauza mfumu ya Isiraeli kuti: "Chonde funsani malangizo kwa Yehova kuti muyambe kuchita chiyani. ⁶ Pamenepo mfumu ya Isiraeli inasonkhanitsa aneneri mazana anai, nanena nao, Ndipite kunkhondo ku Ramoti Giliyadi, kapena ndisapite? Iwo anati, "Umbani, pakuti Yehova adzaupereka m'manja mwa mfumu." ⁷ Koma Yehosafati anati, Kodi pano palibenso mneneri wina wa Yehova amene tingapemphe malangizo kwa iye? ⁸ Mfumu ya Isiraeli inauza Yehosafati kuti: "Pali munthu mmodzi amene tingapemphe malangizo kwa Yehova kuti atithandize, ndiye Mikaya mwana wa Imla, koma ndimadana naye chifukwa salosera zabwino za ine, koma zowawa. Koma Yehosafati anati, Mfumu isatero. ⁹ Kenako mfumu ya Isiraeli inaitana kapitawo wa asilikali n'kumuuza kuti: "Bwera naye Mikaya mwana wa Imla nthawi yomweyo. ¹⁰ Ndipo Ahabu mfumu ya Isiraeli ndi Yehosafati mfumu ya Yuda anakhala yense pa mpando wacifumu, atabvala zobvala zao, pa dwale pa cipata ca Samariya; ndipo aneneri onse anali kunenera pamaso pao. ¹¹ Zedekiya mwana wa Kenaana anadzipangira nyanga zachitsulo n'kunena kuti: "Yehova wanena kuti, 'Ndi nyangazi mudzakantha Aaramu mpaka kuwatha.'" ¹² Aneneri onsewo analosera mofananamo kuti: "Kanthani Ramoti Giliyadi ndipo mudzapambana. Yehova waupereka m'manja mwa mfumu. ¹³ Ndipo mthenga amene anapita kukaitana Mikaya ananena naye, nati, Taona, mau a aneneri anenera zabwino pamodzi ndi mfumu; mau ako akhale ngati amodzi mwa iwo, nunene zabwino. ¹⁴ Mikaya anayankha kuti: "Pali Yehova wamoyo, zimene Yehova wanena kwa ine ndinena. ¹⁵ Atafika kwa mfumu, mfumu inati kwa iye, Mikaya, kodi tipite kunkhondo ku Ramoti Giliyadi kapena tileke? Mikaya anayankha, nati, Menyani ndi kupambana; Yehova adzaupereka m'dzanja la mfumu. ¹⁶ Pamenepo mfumu inati kwa iye, Ndizakulumbiritsa kangati kuti usandiuze zoona zokhazokha m'dzina la Yehova? ¹⁷ Ndipo Mikaya anati, Ndinaona Aisiraeli onse atabalalika kumapiri, ngati nkhoa zopanda mbusa; ndipo Yehova anati, Amenewa alibe mbuye; ¹⁸ Pamenepo mfumu ya Isiraeli inati kwa Yehosafati, Kodi sindinakuuze kuti sadzanenera za ine zabwino, koma zoipa zokha? ¹⁹ Pamenepo Mikaya anati: "Choncho imvani mawu a Yehova: Ndinaona Yehova atakhala pampando wake wachifumu, ndipo khamu lonse lakumwamba litaimirira pambali pake kudzanja lake lamanja ndi lamanzere. ²⁰ Ndipo Yehova anati, Ndani adzanyenga Ahabu, kuti akwere nakagwe ku Ramoti Gileadi? Mmodzi wa iwo ananena izi ndipo wina ananena izo. ²¹ Pamenepo mzimu unadza, nuima pamaso pa Yehova, niti, Ine ndidzam'nyenga. Yehova anati kwa iye, Bwanji? ²² Ndipo mzimuwo unati, Ndizatuluka ndi kudzakhala mzimu wonama m'kamwa mwa aneneri ake onse. Yehova anayankha kuti, 'Udzamunyengerera, ndipo udzapambana. Pita tsopano, ukachite. ²³ Tsopano taonani, Yehova waika mzimu wonama m'kamwa mwa aneneri anu onsewa, ndipo Yehova walamula kuti muchite zoipa." ²⁴ Pamenepo Zedekiya mwana wa Kenaana anakwera, namenya Mikaya patsaya, nati, Mzimu wa Yehova wapita kuti kundichokera kukalankhula nawe? ²⁵ Mikaya anati: "Udzaona tsiku limenelo pamene udzabisala m'chipinda chamkati. ²⁶ Mfumu ya Isiraeli inauza mtumiki wake kuti: "Mgwire Mikaya ndi kupita naye kwa Amoni kazembe wa mzindawo, ndi kwa Yowasi mwana wanga. ²⁷ Amunene kuti, 'Mfumu ikuti, Ikani munthu uyu m'ndende, ndipo mum'patse chakudya cha nsautso ndi madzi a nsautso kufikira ndikadzabwera mwamtendere. ²⁸ Pamenepo Mikaya anati: "Mukabwerera bwinobwino, ndiye kuti Yehova sananene mwa ine. Kenako anawonjezera kuti: "Mverani izi, anthu nonsenu. ²⁹ Choncho Ahabu mfumu ya Isiraeli ndi Yehosafati mfumu ya Yuda anapita ku Ramoti Giliyadi. ³⁰ Mfumu ya Isiraeli inauza Yehosafati kuti: "Ine ndidzisintha ndi kupita kunkhondo, koma iwe vala zovala zako zachifumu. Chotero mfumu ya Isiraeli inadzisintha + n'kupita kunkhondo. ³¹ Ndipo mfumu ya Aramu inalamulira akapitao makumi atatu mphambu awiri a magareta ace, ndi kuti, Musakantha ankondo ang'ono kapena omveka; ³² Ndipo panali pamene akapitao a magareta anaona Yehosafati, anati, Zoonadi, ameneyo ndiye mfumu ya Isiraeli. Iwo anatembenuka kuti amenyane naye, choncho Yehosafati analira. ³³ Ndiyeno akuluakulu a magaletawo ataona kuti si mfumu ya Isiraeli, anabwerera osamuthamangitsa. ³⁴ Koma munthu wina anaponya uta wake mwachisawawa, nalasa mfumu ya Isiraeli pakati pa mfundo za zida zake. Pamenepo Ahabu anauza woyendetsa galeta lake kuti: "Tembenuka unditulutse kunkhondo, pakuti ndavulala kwambiri. ³⁵ Nkhondoyo inakula tsiku lomwelo, ndipo mfumu inaimitsidwa m'galeta lake pamaso pa Aaramu. Iye anafa madzulo. Mwazi unatuluka m'balalo n'kulowa pansi pa gareta. ³⁶ Pamenepo dzuwa linali kulowa, anthu anafuula kuti: "Aliyense abwerere kumudzi wake, ndipo aliyense abwerere kuderu lake. ³⁷ Chotero Mfumu Ahabu anamwalira, ndipo anatengedwa kupita ku Samariya, ndipo anamuika m'manda ku Samariya. ³⁸ Iwo anatsuka gareta pa thamanda la Samariya, ndipo agalu

ananyambita magazi ake (kumeneko n'kumene amahule ankasamba), monga mmene Yehova ananenera.³⁹ Nkhani zina zokhudza Ahabu ndi zonse zimene anachita, nyumba ya minyanga ya njovu imene anamanga ndi mizinda yonse imene anamanga, zinalembedwa m'buku la zochitika za mafumu a Isiraeli kodi?⁴⁰ Choncho Ahabu anagona pamodzi ndi makolo ake, ndipo Ahaziya mwana wake anayamba kulumulira m'malo mwake.⁴¹ Kenako Yehosafati mwana wa Asa anayamba kulumulira Yuda m'chaka chachinayi cha Ahabu mfumu ya Isiraeli.⁴² Yehosafati anali wa zaka makumi atatu kudza zisanu polowa ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka makumi awiri mphambu zisanu. Dzina la amayi ake linali Azuba mwana wa Sili.⁴³ Iye anayenda m'njira za atate wake Asa; sanapatuke kwa iwo; Iye anachita zoyenera pamaso pa Yehova. Koma misanje sinachotsedwe. Anthu anali kuperekabe nsembe ndi kufukiza pamisanje.⁴⁴ Yehosafati anachita mtendere ndi mfumu ya Isiraeli.⁴⁵ Nkhani zina zokhudza Yehosafati ndi mphamvu zimene anachita, ndi mmene anamenyera nkhondo, zinalembedwa m'buku la zochitika za mafumu a Yuda.⁴⁶ Anachotsa m'dziko mahule ena onse amene anatsala m'masiku a bambo ake Asa.⁴⁷ Munalibe mfumu ku Edomu koma wachiwiri wake ankalamulira kumeneko.⁴⁸ Yehosafati anamanga zombo za ku Tarisi; Anayenera kupita ku Ofiri kukatenga golide, koma sanapite chifukwa zombozo zinasweka ku Ezioni Geberi.⁴⁹ Pamenepo Ahaziya mwana wa Ahabu anauza Yehosafati kuti: "Atumiki anga apite limodzi ndi atumiki ako m'zombo. Koma Yehosafati sanalole.⁵⁰ Yehosafati anagona pamodzi ndi makolo ake, naikidwa pamodzi ndi makolo ake mu Mzinda wa Davide kholo lake; Yehoramu mwana wake anakhala mfumu m'malo mwake.⁵¹ Ahaziya mwana wa Ahabu anakhala mfumu ya Isiraeli ku Samariya m'chaka cha 17 cha Yehosafati mfumu ya Yuda, ndipo analumulira Isiraeli zaka ziwiri.⁵² Iye anachita zoipa pamaso pa Yehova, ndipo anayenda m'njira ya bambo ake, m'njira ya mayi ake, ndi m'njira ya Yerobiamu mwana wa Nebati, imene anachimwitsa nayo Isiraeli.⁵³ Iye anatumikira Baala ndi kum'lambira, moti anakwiyitsa Yehova Mulungu wa Isiraeli, monga mmene bambo ake anachitira.

2 Kings

Chapter 1

¹ Moab anapandukila Israyeli ku choka infa ya Ahab. ² Ndiye Ahaziah anagwa pansi nakuzichita chilonda. Mwaicho anatuma batumiki nakubuza, "Yendani, funsani Baal-zebub, mulungu wa Ekron, ngati chizapola chilonda ichi." ³ Koma mungeli wa Yahwe anakamba kuli Elijah mu Tishbite, "Nyamuka, yenda pamwamba kumana na batumiki ba mfumu baku Samaria, naku bafunsa, kuti muyenda kukumana na Baal-Zebub, mulungu waku Ekron?" ⁴ Mwaicho Yahwe anakamba, "Suzabwela pansi ku choka pa bedi pamene unayenda pamwamba; koma, uzafa ndithu." ⁵ Ndipo Elijah anayenda. ⁶ Pamene batumiki bana bwelela kuli Ahaziah, anabuza, "Nichani mwa bwelela?" ⁷ Banakamba kuli eve, "Mwamuna anabwela ku kumana naise anakamba kuli ise, 'Bwelelani kuli mfumu akutumani, na kukamba kuli eve, 'Mulungu akamba ivi: 'Nimchifukwa mulibe Mulungu mu Israyeli kuti mutume bamuna kubnvelana na Baal-Zebub, mulungu wa Ekron? Mwaicho Yahwe anakamba, "Suzabwela pansi ku choka pa bedi pamene unayenda pamwamba; koma, uzafa ndithu." ⁸ Ahaiah anakamba kuli batumiki bake, "Enze mwamuna wa bwanji, wamene anabwela pamwamba ku kumana naimwe na ku kuuzani mau aya?" ⁹ Bana muyanka, "Anavala chopangiwa nasisi ndipo enzeli na belt ya chikumba ku zunguluka mu msana wake." Mwaicho mfumu anayanka, "Ni Elijah mu Tishbite." ¹⁰ Ndiye mfumu anatuma kapteni naba nkondo fifite kuli Elia. Kapten anayenda pamwamba pa lupili pamene anankala Elia. Kapten anakamba kuli eve, "Iwe, mwamuna wa Mulungu, mfumu akamba, 'Bwela pansi.'" ¹¹ Elia anayanka naku kamba kuli kapteni, "Ngati ndine mwamuna wa Mulungu, lekani mulilo ubwele pansi ku shoka iwe nabamuna bali fifite." Ndiye mulilo unabwela pansi ku choka kumwamba naku mu shoka nabamuna bake fifite. ¹² Ndiponso mfumu Ahaziah anatuma kapteni winangu naba nkondo bali fifite kuli Elia. Naye kapteni uyu anakamba kuli Elia, "Iwe mwamuna wa Mulungu, mfumu akamba, "Yendesa bwela pansi." ¹³ Elia anayanka naku kamba kuli beve, "Ngati ndine mwamuna wa Mulungu, lekani mulilo ubwele pansi ku choka ku mwamba naku kushoka na bamuna bali fifite." Nafuti mulilo wa Mulungu unabwela pansi kuchoka kumwamba naku mushoka naba muna fifite. ¹⁴ Nafuti mfumu anatuma gulu ya chitatu yaba nkondo fifite. Uyu kapteni anayenda pamwamba, naku mugwadila pasogolo pa Elia, "Iwe mwamuna wa Mulungu, nikufunsa leka umumoyo wanga na waba nchito bako bali fifite bankale ba bwino pa menso pako. ¹⁵ Nicha zooni, mulilo unabwela pansi ku choka ku mwamba naku shoka ma kapteni yabili pamozi na bamuna bao, koma manje leka moyo wanga unkale wabwino mu menso yako." ¹⁶ Mungeli wa Yahwe anakamba kuli Elia. "Yenda naye. Osachita mantha." Mwaicho Elia anauka naku yenda naye kuli mfumu. ¹⁷ Mukupita kwa nthawi Elia anakamba kuli Ahaziah, "Ivi ndiye vamene Yahwe anakamba, 'Unatuma batumiki ku nvelana na Baal-Zebub, mulungu wa Ekron. Nichifukwa chakuti mulibe Mulungu mu Israyeli kwamenen munga

chose nkani? Sopano, siuzabwela pansi ku choka pa bedi pamene unayenda pamwamba; koma, uzafa ndithu." ¹⁷
Ndiye mfumu Ahaziah anafa monga mwamene mau ya Yahwe yamene anakamba Elia. Joram anayamba kulamulila mumalo yake, mu chaka chachibili cha Jehoram mwana mwamuna wa Jehoshaphat mfumun ya Yuda, chifukwa Ahaziah enzelibe mwana mwamuna. ¹⁸ Pa nkani zina za Ahaziah, sizili olembewa mubuku yazochitika za mfumu za Israyeli?

Chapter 2

¹ Ndipo kunachitika, pamene Yahwe anali kunyamula Elia na kavuluvulu kuyenda naye kumwamba, elia ananyamuka na Elisaha kuchokela ku Gilgal. ² Elia anakamba kuli Elisha, "Napapata, nkhalakuno, chifukwa Yahwe anituma ku Bethel." Elisha anayanaka, "Monga Yahwe anakala, naiwe unkala, siniza kusiya." Mwaicho banayenda ku Bethel. ³ Bana bamuna ba muneneli bamene benzeli ku Bethel bana bwela kuli Elisha nakukamba kuli eve, "Mwati uziba kuti Yahwe azatenga mbuye wanu kuchokela lelo?" Elisha anayanka, "Niziba, koma osavikambapo." ⁴ Elia anakamba kuli eve, Elisha, "Embekeza apa, napapapta, ni ichi Yahwe anituma ku Jeriko." Ndiye Elisha anayanka, "Monga Yahwe ankala, monga naiwe unkala, siniza kusiya." Mwaicho banayenda ku Jeriko. ⁵ Ndiye bana bamuna ba baneneli bamene banayenda pa Jeriko ku bwela kuli Elisha naku kamba kuli eve, "Mwati muiba kuti Yahwe azatenga mbuye wanu kuchoka lelo?" Elisha anayanka, "Nichi ziba ichi, koma osakambapo." ⁶ Ndipo Elia anakamba kuli eve, "Napapata nkala pano ni ichi Yahwe anituma ku Jordn." Monga Yahwe wamoyo, naiwe ndiwe wa moyo, sinizaku siya." Mwaicho bana yenda babili. ⁷ Mukupita mwa nthawi, bana bamuna ba baneneli bali fifite bana imilila pataliko pamene babili bana imilila pa Jordan. ⁸ Elia anatenga chovala chake, nakulunga natem mazi mwamene, msinje unagabika mbali zonse zibili kuti babili ba pite panthaka poyuma. ⁹ China bwela monga ichi, kuchoka pamene bana jumpa kuti Elia akambe kuli Elisha, "Nfunse chamene ninga kuchitile nikalibe kutengewa kuchoka kuliniwe." Elisha anayanka, "Leka muzozo wako ubwele ka bili pali ine." ¹⁰ Elia anayanka, "Wafunsa chintu chovuta. Chosavuta, ngati wani ona pamene nichosewa kuli iwe, ichi chiza chitika kuli iwe, ichi chiza chitika kuli iwe, koma ngati sichinachitike, sichiachitika." ¹¹ Monga mwamene bana pitiliza kuyenda, bana ona, galata wa mulilo nama hosi yamulilo yana bulikila, nichamene chinapatula bamuna babili kunkala pamozi, ndipo Elia anayenda kumwamba na kavuluvulu. ¹² Elisha anona ichi nakulila, "Tate wanga, tate wanga, magaleta ya Israyeli naba muna ba ma hosi!" sana muone futi Elia, ndipo anatenga vovala vake, naku bwelela kuimilila pa Jordan. ¹³ Andoba nyula yapa nthupi ya Elia yamene inagwa, naku bwelelea kuimilila pa Jordan. ¹⁴ Anadyaka pamanzi na nyula ya pa nthupi ya Elia yamene inagwa naku kamba, "Yahwe alikuti, Mulungu wa Elia?" Pamene ana dyokola pa manzi, yana patuka mbali zibili ndipo Elisha ana jumpa. ¹⁵ Pamene bana bamuna ba mneneli bana muona benzo chokela ku Jeriko kumbali kwabo, bana kamaba, "Muzozo wa Elia upumula pali Elisha!" Mwaicho bana bwela kumukumana, naku mugwadila pansi pasogolo pake. ¹⁶ Bana kamba kuli eve, "Ona manje pakati paba nchito bako pali bamuna ba mphanvu bali fifite. Baleke bayende, tifunsa, ndipo usakile mbuye wako, kapena muzozo wa Yahwe wamutebga pamwamba naku mutaila pa mapili olo mu chigwa." Elisha anayanka, "Awe, osabatuma," ¹⁷ Koma pamene bana mupatikiza Elisha mpaka ananvela nsoni, anakamba, "Batumeni." Ndiye bana tuma bamuna bali fifite, nakusakila masiku yatatu, koma sibana mupeze. ¹⁸ Bana bwelela kuli Elisha, eve enzeli ku Jeriko, ndipo anakamba kulibeve, "Sininakuuzeni imwe, 'Osayenda?'" ¹⁹ Bamuna ba malo aya banakamba kuli Elisha, "Ona, tikupempa, mkalidwe wa aya niyo kondelessa, monga mbuye wathu, koma manzi niyoipa na malo siyo balika." ²⁰ Elisha anayanka, "Nileteleni kambale ka nyowani muikepo na soti," Mwaicho bana muletela. ²¹ Elisha anayenda panja ku manzi naku tailapo soti; ndipo anakamba, "Yahwe anakamba izi, 'Nayapolesa manzi aya. Kuchokela nthawi iyi, sikuzankala infana na malo yosa balika.'" ²² Mwaicho manzi yana chilisiwa mpaka lelo, ku mau yamene Elisha anakamba. ²³ Ndipo Elisha anayenda pamwamba kuchoka kuja kuyenda ku Bethel. Mwamene enzoyendela mu road, banyamata bana bwela pamalo naku mudoba; banakamba kuli eve, "Yenda pamwamba iwe wa mutu wapala! Yenda pamwamba wa mutu wapala!" ²⁴ Elisha analangana kumbuyo kwake naku baona; anaitana kuli Yahwe kuti aba tembelele. Ndipo ma gulu yakazi yamu nsanga yana choka naku ba chita vilonda banyamata bali fote. ²⁵ Ndipo Elisha anayenda kuchoka kuja kuyenda kupili ya Carmel, ndipo kuchoka kuja anabwelela ku Samaria.

Chapter 3

¹ Manje muchaka cha eitini cha Jehoshaphat mfumu ya Yuda, Joram mwana mwamuna wa Ahab anayamba kulamulila Israyeli mu Samaria; ana lamulila zaka twovu. ² Anachita voipa pamenso ya Yahwe, koma osati monga batate bake naba mai bake; niichi anachosa chimwala choyofya chamapilala cha Baal chamene banapanga batate bake. ³ Anagwilila machimo ya Jeroboam mwana mwamuna wa Nebat, wamene analengesa Israyeli kuchimwa; sana chokeko kuliyewe. ⁴ Manje Mesha mfumu ya Moab mwana wambelele. Anapasa mfumu waba Israyeli 100,000 bana ba mbelele. ⁵ Koma kucoka pameme Ahab anafela, mfumu ya Moab analeka ku nvelela mfumu ya Israyeli. ⁶ Manje mfumu Joram anachoka ku Samaria nthawi kuti akalimbise Israyeli yonse kuti ichite nkondo. ⁷ Anatuma mau kuli Jehoshaphat mfumu ya Yuda, kukamba, "Mfumu ya Moab yaniukila ine. Uzayenda naine mu nkondo yomenyana na Moab?" Jehoshaphat anayanka, "Nizayenda. Nili mwamene mulili, banthu banu nibanthu banga, mohosi yanga ni mahosi yanu." ⁸ Ndipo anakamba, "Tizamumenya mu njila bwani?" Jehoshaphat anayanka, "Munjila yanu nsanga mwa Edom." ⁹ Mwaicho mfumu waba Israyeli anayenda na mfumu waba Yuda na mfumu waba Edom. Bana zunguluka masiku seveni, ndiponso kunalibe manzi yaba nkondo olo vinyama vinayenda na beve. ¹⁰ Mwaicho mfumu waba Israyeli anakamba, "Nichani ichi? Kodi Yahwe aitana mfumu zitatu kubapasa mumanja mwa Moab?" ¹¹ Koma Jehoshaphat anakamba, "Kulibeko mneneli wa Yahwe pano, kuti tifunse Yahwe kupitila muli eve?" Umozi wa nchito wa mfumu wa Israyeli anayanka naku kamba, Elisha mwana mwamuna wa Shaphat ali pano, wamene anatila manzi pamanja pa Elia." ¹² Jehoshaphat anakamba, "Mau ya Yahwe yali naeve." Mwaicho mfumu wa Israyeli na mfumu wa Edom banayenda naye. ¹³ Elisha anakamba kuli mfumu wa Israyeli, "Nichani cheninga chite naiwe? Yenda kuli mneneli waba tate bako naba mai bako." Mwaicho mfumu wa Israyeli anakamba kuli eve, "Awe, chifukwa Yahwe anaitana ma mfumu yatatu pamozi kuba pasa muma manja mwa Moab." ¹⁴ Elisha anayanka, "Monga Yahwe wamoyo, naimilila pasogolo pake, ngati sinapase ulemu wa Jehoshaphat mfumu wa Yuda, sininga kuikoko nzelu olo naku kulanga. ¹⁵ Koma manje niletele oyimba, "Ndiye ichi chinapita pamene oyimba analiza, kwanja ya Yahweina bwela pali Elisha. ¹⁶ Anakamba, "Yahwe akamba ichi, 'Panga mumana uyu oyuma. ¹⁷ Nichifukwa Yahwe akamba ichi, 'Simuza ona kavuluvulu olo nvula, koma mumana uyu uza zula zula namanzi, ndipo muzamwa, imwe na zibeto zanu na nyama zanu zonse." ¹⁸ Ichi sichintu chovuta pamnso ya Yahwe. Ndiponso azakupasani ulemelelo pali ma Moabite. ¹⁹ Muza menya aliyense olimbisa muzinda na yonse yabwino, mujube chimutengo chili chonse cha bwino, mulekese manzi kuyenda, na kuononga malonyalin yonse ya bwino namyala." ²⁰ Mwaicho kuseni nthawi yo pasa chopeleka kuna bwela manzi kuchokela ku Edom; chalo cnenzeli fulu na manzi. ²¹ Manje pamene bonse ma Moabite kuti mfumu anabwela kuchita ndeo na beve, bana sonkana pamonzi, bonse banakwanisa kuvala vovala va nkondo, ndipo bana imilila pa malile. ²² Bana uka kuseni nazuba yenzeli kusanika pamanzi. Pamene ma Moabite banaona manzi ku mbali kwabo, yana oneka redi monga magari. ²³ Bana punda, "Aya nimagazi! Mafumu yaonongewa, naku payana! Manje, Moab, leka tiyende kuba menya!" ²⁴ Pamene bwela ku msonkano wa Israyeli, ba Israyeli bana nyamuka nakumenya ma Moabite, bana mbuluka pasogolo pabo. Ba nkondo ba Israyeli ku bapisha ba Moabite pakati pa malo. ²⁵ Bana ononga mzinda, napa malo pabwino ponse mwamuna aliyense anatema myala mpaka pana valiwa. Bana lekesa manzi kupita naku juba vimitengo va bwino vonse. Kir Hareseth chabe nde anasala na chi mwala. Koma ma soja ba nkondo navomenyela anabazungulila naku menya. ²⁶ Pamene mfumu wa Moab kuti bana luza ndeo, anatenga bamuna bama naifi bali seveni handiredikuti bangene kuti bangene kuli mfumu wa Edom, koma bana kangiwa. ²⁷ Ndiye anatenga mwana wake mwamuna wamene afunika ku langanile ku choka eve, naku mupasa nsembe yo shoka ku chipupa. Mwaicho kunali ukali pakati paba Israyeli, ndipo ba tuimiki ba Israyeli bana basiya mfumu Mesha naku bwelela ku malo yabo.

Chapter 4

¹ Manje umozi mwana mwamuna wa mneneli mkazi wake na bwelela alila kuli Elisha, kukamba, "Wanchito wanu mwamuna wanga afa, ndipo uziba kuti wanchito wanu enzo yopa Yahwe. Manje bokongolesa babwela kutenga bana banga babili bankale banchito bake." ² Mwaicho Elisha anakamba kuli eve, "Nichani che ninga kuchitile? Niuze unachani munyumba mwako?" Anakamba, alibe chili chonse wanchito wako munyumba koma che poto yama futa." ³ Ndiye Elisha anakamba, "Kapempe ma jah kuli bapafupi bako, muma jah mulibe vili vonse. Pempa yambili monga yeunga pempe." ⁴ Ndiye ungene mukati naku vala chiseko kumbuyo kwako kwako na bana bako, nakutila mafuta muma jah yonse, uchosepo ma jah yazula." ⁵ Mwaicho anamusiya Elisha naku vala chiseko kumbuyo kwake nabana bake. Ndiye banaleta ma jah kuli eve naku ikamo mafuta. ⁶ Pamene vina zula, anakamba kuli mwana wake mwamuna, "Niletele jah inangu." Koma anakamba kuli eve, "Kulibe ma jah yenangu. Ndiye mafuta." Yanaleka kupita. ⁷ Ndiye anabwela naku uza mwana mwamuna wa Mulungu. Anakamba, "Kagulise mafuta; lipila nkongongole yako, nakunkala nabana bako bamuna." ⁸ Siku ina Elisha anayenda ku Shunem kwamene mukazi ana muuza kudya naye. Mwaicho monga kambili enzo pitako Elisha, enzo imilila kudya. ⁹ Mukazi anakamba kuli mwamuna wake, "Ona, manje, nazindikila kuti uyu ni mwana wa Mulungu oyela wamene ama pitililako." ¹⁰ Lekani tipange ka pinda ka Elisha pamwamba pa malata, naku ikamo pogona, tebulo, mupando, na laiti. Ndiwe akabwela kuli ise, azankala paja." ¹¹ Mwaicho pamene siku ina bwela futi kuti Elisha aimilile paja, anankala mu chipinda naku pumuililamo. ¹² Elisha anakamba kuli Gehazi wanchito wake, "Muitane uyu Shunammite." Pamene ana muitana, anaimilila pasogolo pake. ¹³ Elisha anakamba kuli eve, "Kamba kuli eve, 'Wayenda muma vuto yonse kusamalila ise. Nichani chinga kuchitikileni? Tinga ku kambile kuli mfumu olo wolamulila wa nkondo?'" Anayanka, "Ninkala pakati pa banthu banga" ¹⁴ Mwaicho Elisha anakamba, "Nichani che tingamuchitile kanshi?" Gehazi anayanka, "Nimotere, alibe mwana mwa muna, ndipo mwamuna wake ni okota." ¹⁵ Mwaicho Elisha anayanka, "Muitane." Pamene ana muitana, anaimilla pa chiseko. ¹⁶ Elisha anakamba, "Nthawi ino ya chaka, mu nthawi chaka chobwelela, uzagwila mwana mwamuna." Anakamba, "Iyayi, mbuye wanga na mwana wa Mulungu, osamunama wanchito wako." ¹⁷ Koma mukazi anabala nakunkala na mwana mwamuna nthawi yamene ija chaka chokonkapo, monga Elisha ana muuza. ¹⁸ Pamene mwana anakula, siku imozi anayenda panja kuli batate bake, bamene banali nabo lima babo. ¹⁹ Anakamba kuli batate bake, "Mutu wanga, mutu wanga." Batate bake bana kamba kuli ba nchito babo, "Munyamuleni kuli bamai bake." ²⁰ Pamene banchito bake bana munyamula naku peleka mwamuna kuli bamai bake, mwana anankala pama konkola pabo mpaka namuzuba nakufa. ²¹ Mwaicho mukazi ananyamuka naku goneka mwamuna pogona pa munyithu wa Mulungu, anavala door naku choka. ²² Anaitana bamuna bake, naku kamba, "Napapata nitumimeni wa nchito umozi na donkey. Mwaicho kuti niyendese kuli mwana wa Mulungu naku bwelela." ²³ Bamuna bake bana funsa, "Nichani ufuna kuyenda kuli eve lelo? Simwezi yanyowani olo sabata." ²⁴ Ndiye ana kwela pa donkey naku kamba kuli wanchito wake, "Yenza mwa musanga, osa yenza pangono koma ngati naku uza." ²⁵ Mwaicho anayenda naku bwela kuli mwana wa Mulungu pa pili ya Carmel. Manje pamene mwana wa Mulungu ana muonela patali, ana kamba kuli Gehazi wa nchito wake, "Ona, apa bwela mukazi wa Shunammite." ²⁶ Napapata mutamangile naku kamba kuli eve, 'Mwati vonse vili bwino iwe naba muna bako na mwana.'" Anayanka, "Vili bwino." ²⁷ Pamene anabwela kuli mwana wa Mulungu pa lupili, anagwila mendo yake. Gehazi anabwela pafupi na eve kuti amu choseko koma mwana wa Mulungu anakamba, "Muleke, chifukwa niokalipa manigi, na Yahwe abisa vuto kuli ine, ndipo kulibe vamene anniuza." ²⁸ Ndiye anakamba, "Nina ku pempani mwana mwa muna, mbuye wanga? Sini nakamba kambe, 'Kuti osa ninama?'" ²⁹ Ndiye Elisha anakamba kuli Gehazi, "Vala vapa ulendo na kunyamula vintu vanga mumanja mwako. Yenda kunyumba kwake. Ngati wakumana na mwamuna aliyense, osa mmuposha, ndipo ngati aliyense aku posha, osa muyanka ugoneke vintu vanga pa menso pa mwana." ³⁰ Koma mai wamwana anakamba, "Monga Yahwe wamoyo, monga naiwe wa moyo, siniza kuleka." Mwaicho Elisha anaimilila naku mukonka. ³¹ Gehazi anayendesa pasogolo pabo nakugoneka vintu pamnso pa mwana, koma mwamuna sana kambe olo kunvela. Ndiponso Gehazi anabwelela ku kumana na Elisha naku muuza kukamba, "Mwana sana uke." ³² Pamene Elisha anafika panyumba, mwana anali okufa enzeli akali pogona. ³³ Mwaicho Elisha anangena naku vala chiseko pali mwana na eve nakumu pempelela kuli Yahwe. ³⁴ Anayenda pamwamba naku mugenela mwana; anaika kamwa yake pakamwa pake, menso yake pamenso yake ndipo manje yake pa manja pake. Ana ziyondolola pali mwana, ndipo tupi yamwana inathuma. ³⁵ Ndiye Elisha ananyamuka naku zunguluka chipinda naku nyamulka futi naku ziyondolola pali mwana. mwana ana etyemula kali seveni ndiye kusegula menso yake! ³⁶ Mwaicho Elisha anaitana Gehazi naku kamba, "Muitana Shunammite!" Mwaicho anamuitana, ndipo pamene anangena mu chipinda, Elisha anakamba, "Mutenge mwana wako mwamuna." ³⁷ Ndiye anagoneka pamenso pake pansi pa memndo yake nakugwanda pansi, naku munyamula

mwana wake mwamuna nakuyenda panja.³⁸ Ndiye Elisha anabwela futi ku Gilgal. Kwezeli njala mumalo muja, na bana bamuna ba mneneli banali nkale pasogolo pake. Anakamba ku banchito bake, "Ikani poto ikulu pa mulilo naku pika supu yabana bamuna ba baneneli."³⁹ Umozi pali beve anayenda kuika pamozi ndiyo zamatepo. Anapeza vinyu yamusanga nakuika pamozi nongo zamusanga kuzulisa zake. Bana juba na kuika pamozi mu nyama, koma sanazibe mutundu wakayena.⁴⁰ Mwaicho bana tila nyama kuti bamuna badye. Nthawi ing'ono pamene benze kudya, bana lila naku kamba, "Mwana wa Mulungu, muli infa mu poto!" Mwaicho sibanadye nafuti.⁴¹ Koma Elisha anakamba, "Letakoni unga opangila buledi." Anaitila mu poto naku kamba, "Batitile banthu kuti banthu badye." Pamenepo munalibe kanthu kubasausa mumphika.⁴² Mwamuna anachokela ku Ball Shalisha kuli mtumiki wa Mulungu naku bwelesa mikate twenti ya bale mu saka yake kuchokela nthawi yokolola, na ngalata zasopano. Anakamba, "Pasani banthu ivi kuti badye."⁴³ Na wanchito wake anakamba, "Nivichani vamene niza faka pasogolo pali bamuna bali handredi?" Koma Elisha anakamba, "Bapaseni ivi banthu, kuti badye, chifukwa Yahwe akamba, ' Bazadya navinangu ku salako.'" ⁴⁴ Mwaicho banchito bake bana faka pasogolo pabo; banadya, navinangu kusalako, monga mwamene mau ya Yahwe yana lonjeza.

Chapter 5

¹ Manje Naaman, msogoleli waba nkondo wa mfumu Aram, anali mwamuna opambana na olemekeza mulamlanganilo ya mbuye, chifukwa cha eve Yahwe anapasa Aram chigomezo. Komanso anali mwana oumba na olimba mtima, koma anali wakate. ² Ma Arameans bana yenda panja kulimbana nama gulu ndipo banatenga mukazi wachi chepele wapa mzinda wa Israyeli. Ana pulumusa mukazi wa Naaman. ³ Mukazi wachichepele anakamba na mukazi wake waku mbali, "Sembe kapena mbuye wanga anali na mneneli waku Samaria! Ndiye anga polese mbuye wanga ku kate." ⁴ Ndipo Naaman anayenda nakuuza mfumu vamene mukazi wachi chepele ochokela mu malo ya Israyeli. ⁵ Ndipo mfumu wa Aram anakamba, "Yenda manje ndipo nizatuma kalata kuli mfumu wa Israyeli." Naaman anayenda nakutenga ma talanta ya siliva yali teni, ma pisi ya golide yali 6,000 na vovala vochinja vili teni. ⁶ Kamanso anapeleka kalata kuli mfumu wa Israyeli yame inakamba, "Manje pamene kalata yabwela kuli iwe, uzaona kuti natuma Naamani umupolese kate yake." ⁷ Pamene mfumu wa Israyeli anabelenga kalata, anangamba vovala vake nakukamba, "Ine ndine Mulungu kuti nipaya nakupanga moyo, kuti uyu mwamuna afuna nipolese kate yake? Chioneka afuna kayamba mukangano naine." ⁸ Ndipo pamene Elisha mtumiki wa Mulungu ananvela kuti mfumu wa Israyeli ana ng'amba vovala vake, anatuma kuli mfumu kukamba, "Nichani wang'amba vovala vako? Muteke abwele kuli ine, ndipo aza ziba kuti muli mneneli mu Israyeli." ⁹ Ndipo Naaman anabwela nama tavalu nama galata naku imilila pa chiseko pa Elisha. ¹⁰ Elisha anatuma mtumiki kuli eve, kukamba, "Yenda naku zidumbwisa mu Jordan kali seveni, ndipo tupi yako izankla yopepuka; uzankala osalala." ¹¹ Koma Naaman anakalipa naku chokapo naku kamba, "Ona nenzo ganiza azabwela panja kuli ine kuimilila naku itana pazina ya Yahwe Mulungu wake, naku baibisha kwanja yake pamalo ponse naku polesa kate yanga." ¹² Abanah na Pharthar, simi mumana za Damascus, yalipo bwino kuchila ma damu yonse ya Israyeli? Sininga sambemo nakunka osalala?" Ndipo ana pindimuka nakuyenda. ¹³ Ndipo wanchito wa Naaman anabwela pafupi naku kamba naye, "Tate wanga, ngati mneneli akulamulila kuchita chintu chovuta, sunga chi chite? Nanga ichi chavuta bwanji, ngati akamba kuli iwe, 'Zidumbwisilemo naku salala.'" ¹⁴ Ndiye anayenda pansi naku zidumbwisa kali seveni mu Jordan, kunvelela vamene auziwa kuchita kuli mtumiki wa Mulungu. Tupi yake inabwelelamo futi monga tupi yaka mwana kang'ono, ndipo anapola. ¹⁵ Naaman anabwelela kuli mtumiki wa Mulungu, navonse vake, anabwela naku imilila pasogolo pake. Anakamba, "Ona, manje naziba kuti kulibe Mulungu mu chalo chonse koma mu Israyeli, tenga mphaso kuchokela kuli wanchito wako." ¹⁶ Koma Elisha anayanka, "Monga Yahwe wamoyo, pasogolo pake naimilila, siniza pokelela chili chonse." Naaman ana patikiza Elisha kutenga mphaso, koma anakana. ¹⁷ Pamenepo Naaman anakamba, "Ngati siconcho nikupempani kuti mtumiki wanu apisiwa mtolo wa kuyambila manje, ine mtumiki wanu sinizapeleka nsembe yoshoka kwa Mulungu wina koma Yahwe." ¹⁸ Muli ichi chimozi ileke Yahwe aleke wanchito wako, kuti, ngati mfumu wanga angena mu nyumba ya Rimmon kupembeza kuja, naku samila pa kwanja panga, ndipo nizagwala mu nyumba mwa Rimmon, pamene nagwada mu nyumba mwa Rimmon, lekani Yahwe akukululukile iwe wanchito pankani iyi." ¹⁹ Elisha anakamba kuli eve, "Yenda mumtendele." Mwaicho Naamna anayenda. ²⁰ Anayenda ulendo wapafupi chabe, pamene Gehazi wanchito wa Elisha mneneli wa Mulungu anakamba eka, "Ona, mbuye wanga anamulekelela uyu Naaman wa Aramean kusapokelela mpaso zamu manja mwake zamneen analeta kuli eve. Monga Yahwe wamoyo, niza mukonka na tenga chintu kuli eve." ²¹ Mwaicho Gehazi anakonkamo Naaman. Pamene Naaman anaona munthu amutangila, ana jumpa pansi kuchoka pama galata ku kumana na eve naku kumba, "Mati zonse zili bwino?" ²² Gehazi anakamba, "Vonse vili bwino. Mbuye wanga anituma, kukamba, 'Ona, manje babwela kuliine kuchoka ku ziko yamapili ya Ephraim anyamata babili bana ba mneneli napapata bapeseni matalanta yasiliva na vovala vibili.'" ²³ Naaman anayanka, "NNdine okwondwela manigi kupasani matalanta yabili." Naaman anapatikiza Gehazi na kumanga ma talanta yabili yasiliva mumachola yabili, na vovala vochinja vibili, naku vigoneka pa banchito bake babili, bamene bananyamula ma chola ya siliva pasogolo pa Gehazi. ²⁴ Pamene Gehazi anabwela kupili, anatenga machola ya siliva mu manja mwabo naku yabisa mu nyumba, anabapisha bamuna, ndipo bana yenda. ²⁵ Pamene Gehazi anayenda naku imilila pasogolo pa mbuye wake, Elisha anakamba kuli eve, "Wachokela kuti, Gehazi?" Anayanka, "Wanchito wako kulibe kwamene anayenda." ²⁶ Elisha anakamba kuli Gehazi, "Muzozo wanga siwenzeli naimwe pamene mwamuna wanga anapindamula ma ngalata yake ku kumana naiwe? Kodi ni nthawi yovomela ndalama na vovala, madimba ya oliva na pesa, mbelele na ng'ombe imuna, banchito bamuna na banchito bakazi." ²⁷ Mwaicho kate wa Naaman uzankala pali iwe na mbadwa wako wamuyaya."

Chapter 6

¹ Bana bamuna ba mneneli bana kamba kuli Elisha, "Pamalo pamene tinkala iwe naise tonse ni pan'ono manigi. ² Leka tiyende ku Jordan tapapta, ndipo uleke mwamuna aliyense ajube mutengo, naku tileka timange malo yonkalapo kuja kwamene tingankale." Elisha anayanka, "Munga yende." ³ Umozi pali beve anakamba, "Yenda naba nchito bako." Elisha anayanka, "Nizayenda." ^{4 5} Mwaicho anayenda nabo, ndipo pamene banabwela ku Jordan, banayamba kutema mitengo. Koma pamene umozi anali kujuba, analila naku kamba, "Iye mbuye wanga chinali chopempa!" ⁶ Mwaicho mneneli anakamba, "Chagwela pati?" Mwamuna analangiza Elisha pa malo. Ndipo anajuba ka mtengo, ku kataila mu manzi, nakulegesa chisulo kubwela pamwamba pa manzi. ⁷ Elisha anakamba, "Chi dobe." Ndipo mwamuna ana pitisa kwanja yake nakutenga. ⁸ Manje mfumu wa Aram enzo chita ndeo kuli ba Israyeli. Ana nvelana naba nchito bake, kukamba, "Musonkano wanga uzunkala so na malo ya so." ⁹ Mwaicho mtumiki wa Mulungu anatuma kuli mfumu wa Israyeli, kukamba, "Chenjela osapita ku malo aya, chifukwa ma Aramean bayenda kwamene kuja." ¹⁰ Mfumu wa Israyeli anatuma mau ku malo yamene mtumiki wa Mulungu anakamba naku muchenjeza. Kuchila kamozi olo kabili, pamene mfumu anayenda kuja, enzeli ku londewa. ¹¹ Mfumu Aram anakalipisiwa nama chenjezo aya, ndipo anaitana banchito bake naku kamba kuli beve, "Simuzani uza pakati paise wamene ali kumbali kuli mfumu wa Israyeli?" ¹² Mwaicho umozi pali banchito bake anakamba, "Awe mbuye wanga, mfumu, chifukwa Elisha mneneli wa Israyeli amauza mfumu wa Israyeli amakamba vamene mumakamba mu chipinda mwanu." ¹³ Mfumu anayanka, "Yendani muone kwamene ankala Elisha kuti ninga tume bamuna kumugila." Anauziwa, "Ona, ali mu Dothan." ¹⁴ Mwaicho mfumu anatuma ma hosi, magalata naba nkondo bambili. Banabwela usiku nakuzunguluka malo. ¹⁵ Pamene banchito ba mtumiki ba Mulungu bana uka uka kuseni nakuyenda panja, ona, ba nkondo bambili nama hosi na magalata bana zunguluka malo. Wanchito wake anakamba kuli eve, "Iye mbuye wanga! Tizachita chani?" ¹⁶ Elisha anayanka, "Osayopa, chifukwa bamene bali naise bali bambili kuchila bali nabeve." ¹⁷ Elisha ana pempela naku kamba, "Yahwe nipempa mu musegule menso kuti aone." Ndiye Yahwe anasegula menso ya wanchito ndipo anaona. Onani, lupili inalifulu nama kavalo na mgalata kuzungulika Elisha! ¹⁸ Pamene ma Arameans yanabwela pansi kuli eve, Elisha ana pempela kuli Yahwe naku kamba, "Ba pangenji mpofu bantu aba nikupempani." Mwaicho Yahwe ana bapanga mpofu munga mwamene Elisha anapempa. ¹⁹ Ndiye Elisha anauza ma Arameans, "Iyi, sinjila, kapena malo. Nikonke ndipo nizakuletani kuli mwamuna wamene musakila." Ndiye anaba sogolela ku Samria. ²⁰ Chinabwela chakuti pamene bana bwela mu Samaria, Elisha anakamba, "Yahwe segulani menso yaba muna aba kuti bangone." Yahwe anasegula menso yabo banaona, na Onani, banali pakati pa malo ya Samaria. ²¹ Mfumu wa Israyeli anakamba kuli Elisha, pamene anabaona, "Tate wanga, niba paye? Niba paye?" ²² Elisha anayanka, "Musa bapaye. Kodi unga paye bamene wagwila nabemba yako naku gwada? Ba pasaeni mukatenna manzi beve, kuti badye nakumwa, ndipo bayende kuli mbuye wao." ²³ Mwaicho mfumu anakonza vokudya vabo vambili, ndipo pamene banamwa nakumwa anapisha, naku bwelela kuli mbuye wabo. Ija gulu yaba nkondo baku Aramean sibana bwelele nthawi itali mumalo ya Israyeli. ²⁴ Pambuyo pake uyu Ben Hadad mfumu wa Aram bana kumana naba nkondo bake bonse naku menya ba Samaria na kuizunguluka. ²⁵ Mwaicho panali njala yaikulu ku Samaria, taonani, azangulila mzinda uyu mpaka bulu mukulu azagulisiwa na ndalama zasiliva makumi asanu ndi atatu, na cha chinai cha munkola yakunda matuvi na siliva. ²⁶ Pamene mfumu wa Israyeli enze kupita pa chipupa, mukazi analila kuyli eve, kukamba, "Tandiza mbuye wanga, mfumuy wanga." ²⁷ Anakamba, "Ngati Yahwe sana kutandize ninga kutandize bwanji? Kulikochili chonse chamene chi chokela popuntila kapena mopenolela pesa?" ²⁸ Mfumu anapitiliza, "Nichanoi chamene chiku vita?" Anayanka, "Uyu mukazi anakamba kuli ine, 'Pasa mwana wako mwamuna kuti tumudye lelo, ndipo tizadya mwana wanga mwamuna mailo.'" ²⁹ Ndipo tina mupika naku mudya mwana wanga mwamuna, ndipo nina muuza pa siku yokonkapo, "Pasa mwana wako mwamuna kuti tumudye, koma anamubisa mwana wake mwamuna." ³⁰ Ndipo pamene mfumu ananvela mau ya mukazi, anayamba vovala vake (manje anali kupita pa chipupa), ndipo banthu bana langana nakuona kuti anavala masaka, kutupi yake. ³¹ Ndipo anakamba, "Mulungu anilange mobilikiza, ngati mutu wa Elisa wa safati unkale pakem lelo." ³² Koma Elisha anali nkale munyumba mwake naba kulu bana naye. Mfumu anatuma mwamuna kuchoka pasogolo pake, koma pamene mtumiki anabwela kuli Elisha, anakamba kuli bakulu, "Onani uyu mwana wa muna wa paya atuma kuti atenga mutu wanga? Onani pamene mtumiki azabwela, valani chiseko, na kugwila naku vala chiseko. Kodi sikubveka kwamendo ya mbuye wake kumboyoy kwake?" Pamene enzeli akali kukamba nabeve, mtumiki anabwela pansi kuli eve. ³³ Mfumu anakamba, "Onani, kuvutika uku kuchokela kuli Yahwe. Nichani chamene nizayembekezela Yahwe?"

Chapter 7

¹ Elisha anakamba, "Nivela mau ya Yahwe. Ichi ndiye chamene akamba Yahwe: 'Mailo monga nthawi zino muyeso wa unga opangila mukate wabwino uzaguliswa pa sekeli na miyeso ibili ya belele pachipata cha Samaria.'" ² Pamenepo oyanganila kwanja yake azanka munthu wa Mulungu, nati, onani angankale Yahwe akapange mawindo kumwamba, mwati ivi vingacitike?" Elisha anayanka kuti, "Uzatamba vichitika na menso yako, koma simuzadya kanthu." ³ Manje panja papolobela mumzinda panali bamuna bali foo bezeli nama khate. Bana kambisa beka beka, "Nichani chamene tizankalila kuno panka tife?" ⁴ Ngati takamba kuti tiyende mu mzinda, pamenepo njala ili mzinda ndipo tiza fela mwamene muja. Koma tikankala chabe pano tizafa. Manje tiyeni tiyende ku gulu ya nkondo ya Aramean. Ngati bazatisunga ba moyo, tizankala ba moyo, ndipo bakatipaya tizafa." ⁵ Pamenepo anauka mu mazulo kuti angene mu msonkano wa Aramean; anafika kumapeto kwenikweni kwa msaso anapeza kuti palibe munthu. ⁶ Nichifukwa Mulungu anapanga bankondo ba Aramean kunvela chongo cha magalata, nachongo cha matavala - chongo chinangu cha chongo chinangu cha bankondo, bambili, ndipo bana kambisana, "Mfumu wa Israyeli yanvelana na mafumu yaku Hittites na Egypto kutiukila ise." ⁷ Ndiye bankondo bana ima naku mbululuka kumazulo; bana siya ma tenti yabo, makavalo yabo, mabulu yabo, na msonkano monga mwamene yenzeli, naku tamanga mopulumusa moyo wabo. ⁸ Pamene bamuna bakhate banabwela kumbali ya msonkano, banayenda mu tenti imozi na kudya na kumwa, ndi kutenga siliva na golide na vovala, nakuyenda ku vibisa. Banabwelela naku ngena mu tenti inangu ndipo banatenga vintu vosiyana siyana kuja, ndipo bana vibisa. ⁹ Ndiye bana kambisana, "Sitichita vabwino. Iyi nisiku ya nkani yabwino, koma tinkala zee pali yeve. Ngati tizayembekeza mpaka siku kubwela, chilango chizabwela paliise. Manje, bwelani, lekani tiyende na kuuza nyumba ya mfumu." ¹⁰ Mwaicho banayenda naku itana bapa chiseko chamuzinda. Bana bauza, kukamba, "Teze tianyenda ku msonkano waba Aramean, koma kwenzelibe munthu aliyense na chongo cha aliyense, koma kwezeli ma hosi yomangililiwa, nama bulu yo mangililiwa nama tenti mwamene mweyenzelili. ¹¹ Ndipo bapa chiseko bana punda pali nkani, ndipo inauziba mukati mwa munyumba ya mfumu. ¹² Ndipo mfumu anauka usiku naku kamba kuli banchito bake, "Niza ku uzani vamene ma Aramean bana chita kuli ise. Baziba kuti ndise okalipa, mwaicho banachoka musonkano naku bisama mu munda. Banakamba, 'Bakachoka panja pa mzinda, tizabatenga ba moyo, naku ngena mumzinda.'" ¹³ Umozi waba nchito wa mfumu anayanka naku kamba, "Nikupempalela, bamuna benangu batenge makavalo yali faivi yaza salapo, yamene yasala mu mzinda. Bali monga magulu yabanthu baku Israyeli bamene banyenda - bambili bana nafa nakufa manje; lekani titum ¹⁴ Koteri iwo anatenga magaleta awiri ndi akavalo, ndipo mfumuyo inawatumiza iwo kutsata gulu lankhondo la Aaramu, nati, "Pitani mukawone." ¹⁵ Anawatsatira mpaka kukafika ku Yorodano, ndipo njira yonse inali yodzaza ndi zovala ndi zida zomwe Aaramu anataya mofulumira. Choncho amithenga aja anabwerera kukauza mfumu. ¹⁶ Anthuwo anapita kukafunkha msasa wa Aaramu. Choncho ufa wosalala unagulitsidwa pa sekeli, ndi miyezo iwiri ya barele ndi sekeli, mogwirizana ndi mawu a Yehova. ¹⁷ Mfumu idalamula kapitawo yemwe adatsamira dzanja lake kuti aziyang'anira chipata, ndipo anthu adamupondereza pachipata. Adamwalira monga adanenera munthu wa Mulungu, yemwe adayankhula pomwe mfumu idatsikira kwa iye. ¹⁸ Ndipo kudatero monga munthu wa Mulungu adanena kwa mfumu, kuti, Nthawi ngati iyi chipata cha Samariya chidzakhala ndi miyeso iwiri ya barele ndi sekeli, ndi muyeso umodzi wa ufa ndi sekeli. ¹⁹ Woyang'anira wamkuluyo adayankha munthu wa Mulungu nati, "Onani, ngakhale Yehova atapanga mawindo kumwamba, kodi izi zingachitike?" Elisa adati, "Udzionera ndi maso ako, koma osadya kanthu." ²⁰ Izi n'zimene zinamuchitikira, chifukwa anthu anam'ponda pachipata ndipo anamwalira.

Chapter 8

¹ Tsopano Elisa analankhula ndi mkazi amene anaukitsa mwana wake wamwamuna. Iye anati kwa iye, "Nyamuka, pita ndi banja lako, ndipo ukakhale kwina kulikonse kumene ungathe, m'dziko lina, chifukwa Yehova wayitanitsa njala yomwe idzabwere m'dziko lino kwa zaka zisanu ndi ziwiri." ² Ndipo mkaziyo anauka namvera mau a munthu wa Mulungu. Anapita ndi banja lake ndipo anakhala m ofdziko la Afilisti zaka zisanu ndi ziwiri. ³ Ndipo kunali, zitatha zaka zisanu ndi ziwirizi, mkaziyo anabwerera kuchokera kudziko la Afilisti; ndipo ananka kwa mfumu kukam'pemphepera nyumba yake ndi munda wake. ⁴ Tsopano mfumu inali ikulankhula ndi Gehazi mtumiki wa munthu wa Mulunguyo kuti, "Chonde ndiuzeni zazikulu zonse zimene Elisa wachita." ⁵ Ndipo pamene amafotokoza mfumu momwe Elisa adaukitsira mwana amene wamwalayo, mkazi yemwe mwana wake wamwamuna uja wamukitsa kuti apemphe mfumu nyumba yake ndi munda wake. Gehazi anati, "Mbuye wanga mfumu, uyu ndiye mkazi, ndipo uyu ndi mwana wake, amene Elisa anamuukitsa." ⁶ Mfumuyi itafunsa mayiyo za mwana wake, adamufotokoza. Ndipo mfumu inalamulira kazembe wina za iye, nati, Um'patse cinthu cace conse, ndi zokolola zonse za m'minda yace, kucokera tsiku lomwe anacoka kuthengo kufikira tsopano. ⁷ Elisa anafika ku Damasiko kumene Ben Hadad mfumu ya Aramu anali kudwala. Mfumu idauzidwa kuti, "Munthu wa Mulungu wafika kuno." ⁸ Pamenepo mfumu inauza Hazaeli kuti: "Tenga mphatso, upite nayo kukakumana ndi munthu wa Mulunguyo, ndipo upemphe nzeru kwa Yehova kudzera mwa iye kuti, 'Kodi ndichira matenda angawa?'" ⁹ Pamenepo Hazaeli anapita kukakumana naye ndipo anatenga mphatso naye chilichonse chabwino chilichonse cha ku Damasiko, chotengedwa ndi ngamila makumi anayi. Ndipo Hazaeli anadza, naimirira pamaso pa Elisa, nati, Mwana wanu Beni-Hadadi mfumu ya Aramu wandituma kwa inu, kuti, Kodi ndidzachira matenda angawa? ¹⁰ Elisa anati kwa iye, "Pita ukawuze Ben-Hadadi kuti, 'Uchira ndithu,' koma Yehova wandiwuza kuti adzafa." ¹¹ Pamenepo Elisa anayang'ana Hazaeli mpaka anachita manyazi, ndipo munthu wa Mulungu analira. ¹² Hazaeli anafunsa kuti, "Chifukwa chiyani mukulira mbuyanga?" Iye anayankha kuti, "Chifukwa ndikudziwa choipa chimene udzachitire Aisraeli. Udzawotcha malo awo achitetezo, ndipo udzapha anyamata awo ndi lupanga, ndi kuduladula tiana tawo ndi kutumbula amayi awo omwe ali ndi pakati. akazi." ¹³ Hazaeli anayankha, "Ndani kapolo wanu kuti achite zazikulu izi? Ndi galu chabe." Elisa anayankha, "Yehova wandiwonetsa ine kuti udzakhala mfumu ya Aramu." ¹⁴ Kenako Hazaeli anachoka kwa Elisa n'kupita kwa mbuye wake, ndipo mfumu inamufunsa kuti, "Kodi Elisha wakuuza chiyani?" Iye adayankha, "Adandiuza kuti mudzachira." ¹⁵ Kenako, tsiku lotsatira Hazaeli anatenga bulangete lija naliviika m'madzi, ndipo analiyala pankhope ya Ben Hadad mpaka kumwalira. Kenako Hazaeli anayamba kulamulira m'malo mwake. ^{16 17} Mchaka chachisanu cha Yehoram mwana wa Ahabu, mfumu ya Israeli, Yehoram anayamba kulamulira. Iye anali mwana wa Yehosafati mfumu ya Yuda. Iye anayamba kulamulira pamene Yehosafati anali mfumu ya Yuda. Yehoram anali ndi zaka 32 pamene anayamba kulamulira, ndipo inalamulira zaka zisanu ndi zitatu ku Yerusalemu. ¹⁸ Yehoram anayenda m waysnjira za mafumu a Israeli, monga momwe ankachitira banja la Ahabu. popeza anali ndi mwana wamkazi wa Ahabu akhale mkazi wake; nachita zoipa pamaso pa Yehova. ¹⁹ Komabe, chifukwa cha mtumiki wake Davide, Yehova sanafune kuwononga Yuda, popeza anali atamuwuza kuti adzamupatsa zidzukululu nthawi zonse. ²⁰ M'masiku a Yehoram, Aedomu anapandukira Yuda, ndipo anadziikira mfumu. ²¹ Kenako Yehoram anapita ku Zairi ndi magaleta ake onse. Aedomu atamuzungulira Yehoram, oyang'anira magaleta ake ananyamuka ndi kuwathira nkondo usiku. koma gulu la nkondo la Yehoram linathawa ndi kubwerera kwawo. ²² Choncho Aedomu anapandukira Yuda mpaka lero. Libina nayenso anagalukira nthawi yomweyo. ²³ Nkhani zina zokhudza Yehoram ndi zonse zimene anachita, zinalembedwa m'buku la zochitika za mafumu a Yuda. ²⁴ Yehoram anagona pamodzi ndi makolo ake ndipo anaikidwa m'manda mu Mzinda wa Davide. Kenako Ahaziya + mwana wake anayamba kulamulira m'malo mwake. ²⁵ M'chaka cha 12 cha Yehoram mwana wa Ahabu, mfumu ya Israeli, Ahaziya mwana wa Yehoram mfumu ya Yuda, anayamba kulamulira. ²⁶ Ahaziya anali wa zaka makumi awiri mphambu ziwiri polowa ufumu wace; inalamulira chaka chimodzi ku Yerusalemu. Amayi ake anali Ataliya; anali mwana wamkazi wa Omuri, mfumu ya Israeli. ²⁷ Ndipo Ahaziya anayenda m'njira za nyumba ya Ahabu; Iye anachita zoipa pamaso pa Yehova, + monga momwe anachitira a m'nyumba ya Ahabu, chifukwa Ahaziya anali mpongozi wa banja la Ahabu. ²⁸ Ahaziya anapita ndi Yoram mwana wa Ahabu kukamenyana ndi Hazaeli mfumu ya Aramu ku Ramoti Giliyadi. Asiriya anavulaza Yehoram. ²⁹ Mfumu Yoram inabwerera kukachira ku Yezereeli zilonda zomwe Aaramu anamupatsa ku Rama pamene ankamenyana ndi Hazaeli mfumu ya Aramu. Choncho Ahaziya mwana wa Yehoram mfumu ya Yuda anapita ku Yezereeli kukaona Yehoram mwana wa Ahabu, chifukwa Yoram anali atavulazidwa.

Chapter 9

¹ Mneneri Elisa anaitana mmodzi mwa ana a aneneri nati kwa iye, "Vala zovala, ndipo tenga botolo la mafuta ili m yourdzanja lako upite ku Ramoti Giliyadi. ² Ukalowe ukamuitse pakati pa anzake, ndipo umuperekeze kuchipinda chamkati. ³ Kenako utenge botolo la mafuta ndi kuthira pamutu pake ndi kunena kuti, 'Yehova wanena kuti: "Ndakudzoza iwe kukhala mfumu ya Isiraeli. . "'Kenako tsegula chitseko, n kuthawa, osazengereza." ⁴ Koteri mnyamatayo, mneneri wachinyamatayo, anapita ku Ramoti Giliyadi. ⁵ Atafika kumeneko, anapeza atsogoleri a asilikali atakhala pansi. Chifukwa chake mneneri wachichepereyo adati, "Ndabwera kwa inu, kapitawo." Yehu anayankha, "Ndani wa ife?" Mneneri wachichepereyo adayankha, "Kwa inu, wamkulu." ⁶ Pamenepo Yehu ananyamuka nalowa m'nyumba, ndipo mneneriyo anathira mafuta pamutu pake, nati kwa Yehu, Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, Ndakudzoza iwe ukhale mfumu ya anthu a Yehova, ndi Israyeli. ⁷ Uphe banja la Ahabu mbuye wako kuti ndibwezere magazi a atumiki anga aneneri ndiponso magazi a atumiki onse a Yehova amene anaphedwa ndi Yezebeli. ⁸ Pakuti banja lonse la Ahabu lidzatha, ndipo ndidzapha Ahabu mwana wamwamuna aliyense wamwamuna, kaya ndi kapolo kapena mfulu. ⁹ Ndidzachititsa nyumba ya Ahabu kukhala ngati nyumba ya Yerobowamu mwana wa Nebati ndiponso ngati nyumba ya Baasa mwana wa Ahiya. ¹⁰ Agalu adzadya Yezebeli ku Yezreeli, ndipo sipadzakhala womuyika. "Pamenepo mneneriyo anatsegula chitseko nathawa. ¹¹ Kenako Yehu anatuluka n'kupita kwa antchito a mbuye wake, ndipo munthu wina anamufunsa kuti: "Kodi zili bwino? Yehu anayankha kuti, "Mukumudziwa munthuyo, ndi mtundu wa mawu ake." ¹² Iwo adati, "Ndi uthambi. Tiudze." Yehu anayankha kuti: "Anena ndi ine zakutizakuti, ndiponso anati, 'Atero Yehova: Ndakudzoza iwe kuti ukhale mfumu ya Isiraeli.'" ¹³ Kenako aliyense wa iwo anavula msanga chovala chake chakunja ndi kuchiika pansi pa Yehu pamwamba pa masitepe. Iwo anaimba lipenga ndipo anati, "Yehu ndi mfumu." ¹⁴ Momwemo Yehu mwana wa Yehosafati mwana wa Nimisi anakonzera chiwembu Yoram. Tsopano Yoram anali kuteteza Ramoti-giliyadi, iye ndi Aisiraeli onse, chifukwa cha Hazaeli mfumu ya Siriya. koma Mfumu Yehoram anali atabwerera ku Yezreeli kuti akachiritsidwe mabala amene Aaramu anamupatsa, pomenyana ndi Hazaeli mfumu ya Aramu. ¹⁵ Pamenepo Yehu anauza atumiki a Yoram kuti: "Ngati mukuganiza choncho, musalole aliyense kuti apulumuke ndi kutuluka mumzinda kuti akapite kukanena nkhanu imeneyi ku Yezereeli." ¹⁶ Choncho Yehu anakwera galeta lake kupita ku Yezereeli. pakuti Yoram anali kupumula pamenepo. Tsopano Ahaziya mfumu ya Yuda anali atabwera kudzaonana ndi Yehoram. ¹⁷ Mlonda anali ataimirira pa nsanja ku Yezreeli, ndipo anaona gulu la Yehu likubwera patali; adati, "Ndikuwona gulu la amuna likubwera." Yoram anati, "Tenga wokwera pakavalo, ndipo umutume kukakumana nawo; umuize kuti anene, 'Mukubwera mwamtendere?'" ¹⁸ Koteri munthu anatumizidwa atakwera pahatchi kukakumana naye; iye anati: "Mfumu yanena kuti, 'Kodi mukubwera mwamtendere?'" Yehu anayankha kuti: "Uli ndi chiyani ndi mtendere? Kenako mlondayo anauza mfumu kuti, "Mthengayo wakumana nawo, koma sabwerako." ¹⁹ Kenako anatumizanso munthu wina wachiwiri wokwera pahatchi, amene adadza kwa iwo nati, "Mfumu yanena izi: 'Kodi mukubwera mwamtendere?'" Yehu anayankha kuti, "Uli ndi chiyani ndi mtendere? Tembenuka ukwere kumbuyo kwanga." ²⁰ Mlondayo ananenanso kuti, "Wakumana nawo, koma sabwerako; pakuti akuyendetsa galeta momwemo, ndi momwe Yehu mwana wa Nimshi amayendetsera; akuyendetsa bwino." ²¹ Koteri Yoram anati, "Konzani galeta langa." Anamanganso galeta lake ndipo Yoram mfumu ya Isiraeli ndi Ahaziya mfumu ya Yuda ananyamuka, aliyense pagaleta lake kukakumana ndi Yehu. Anamupeza pamalo a Naboti Myezereeli. ²² Yoram ataona Yehu anati, "Kodi wabwera mwamtendere, Yehu?" Iye anayankha, "Mtendere uli pati, pamene zachiwerewere ndi ufiti za amayi ako Yezebeli zachuluka?" ²³ Comweco Yoram anatembenusa garetu lace nathawa, nanena kwa Ahaziya, Ahabu ali ndi chinyengo. ²⁴ Kenako Yehu anakoka uta ndi mphamvu yake yonse, ndipo analasa Yoram pakati pa mapewa ake. muvi unadutsa mumtima mwake, ndipo anagwa m'gareta wake. ²⁵ Ndipo Yehu anati kwa Bidkara kapitawo wake, "Mnyamule ukamuponye ku munda wa Naboti Myezereeli. Ganizira momwe iwe ndi ine tinakwera pamodzi pambuyo pa Ahabu abambo ake, Yehova anati ulosiwu pa iye:" ²⁶ Dzulo ndinawona magazi za Naboti ndi magazi a ana ake, "watero Yehova," ndipo ndidzakulipiritsa pa munda uno, "watero Yehova. + Tsopano mutenge, mum'ponye pamunda uno, mogwirizana ndi mawu a Yehova." ²⁷ Ahaziya mfumu ya Yuda ataona izi, anathawa m thenjira yopita ku Beti Hagani. Koma Yehu anam'tsatira, nati, Muphenso iye m'gareta; Ahaziya anathawira ku Megido ndipo anafera komweko. ²⁸ Atumiki ake ananyamula mtembo wake ndi galeta kupita nawo ku Yerusalemu ndipo anamuyika m inmanda ake pamodzi ndi makolo ake mu Mzinda wa Davide. ²⁹ M itchaka cha khumi ndi chimodzi cha Yehoram mwana wa Ahabu, Ahaziya anayamba kulamulira Yuda. ³⁰ Yehu atafika ku Yezereeli, Yezebeli anamva zimenezi, ndipo anapaka maso ake, anakonza tsitsi lake, nasuzumira pawindo. ³¹ Yehu akulowa pa chipata, ndipo anati kwa iye, "Kodi ukubwera mwamtendere, Zimiri, wakupha mbuye wako?" ³² Yehu anayang'ana pawindo ndipo anati, "Ndani ali kumbali yanga? Ndani?" Ndipo adindo awiri

kapena atatu anayang'ana kunja. ³³ Ndipo Yehu anati, "Mponye pansi." Choncho anamuponyera pansi Yezebeli, ndipo magari ake ena anawaza pa khoma ndi mahatchi ndipo Yehu anamupondaponda. ³⁴ Yehu atalowa m'nyumba yachifumu, anayamba kudya ndi kumwa. Ndipo anati, Tawonanitu kwa mkazi wotembereredwa uyu, mumuike m'manda, chifukwa ndiye mwana wamkazi wa mfumu. ³⁵ Anapita kukamuika maliro, koma osampeza koma chigaza, mapazi, ndi zikhatho za manja ake. ³⁶ Choncho anabwerera ndi kukauza Yehu. Iye anati, "Awa ndi mawu a Yehova amene anayankhula kudzera mwa mtumiki wake Eliya Mtisibe, kuti, 'M'dziko la Yezreeli agalu adzadya mnofu wa Yezebeli, ³⁷ ndipo thupi la Yezebeli lidzakhala ngati ndowe pamwamba pa minda ya m atdziko la Yezreeli, kotero kuti palibe amene adzanene kuti, "Uyu ndi Yezebeli." "'

Chapter 10

¹ Manje Ahab anali na bobadwa mumbuyo bali sevente mu Samaria. Yehu analemba ma kalata naku yatuma ku Samaria, kuli Jezreel, pamozi bakulu na bo yanganilapo ba Ahab bobadwa mumbuyo, kukamba, ² " Bobadwa mumbuyo ba mbuye banu bali naimwe, ndipo muli nanso na magaleta, nama kavalo nabo limbisa malo na mzinda na chovala ndiponso pamene kalata iza fika kuli imwe, ³ sanakani babwino manigi na woyela pali bo badwa mumbuyo mwa mbuye banu naku pampando wa ufumu wa ba tate bake, naku menyanila mzera zachifumu za ambuye banu." ⁴ Koma bana chita manta naku kamba pakati pawo, "Onani, mafumu yabili yakangiwa kuimilila pasogolo pa Jehu. Chakuti tiza imilila bwanji?" ⁵ Pamene apo mwamuna anali kuyanganila nyumba ya mfumu wamene anali pamalo ponse, naba kulu bonse, ndipo bamene ba kulisa bana, banatuma mau kuli Jehu, kukamba, "Ndise ba nchito banu. Tiza chita vonse vamene mwatilamulila. Sititza ika mwamuna aliyense kunkala mfumu chitani vabwino mu menso mwanu." ⁶ Pamene apo Jehu analemba kalata ka chibili kulibenve, kukamba kuti, "Ngati muli ku mbali kwanga, ndipo ngati muza nvelella mau yanga, mutenge mutu zaba muna za mbadwa za mbuye banu, naku bwela kuli ine mailo ku Jeziri mailo ino ntau." Manje mbadwa za mfumu, bali sevente banli naba muna bofunika bamu malo, bamene benzo baleta pamwamba. ⁷ Chakuti pamene kalata ina bwela kuli benve, bana bamuna ba mfumu naku ba paya, bantu bali sevente, kufaka mitu zabo muma basikete, naku yatuma kuli Jehu mu Jeziri. ⁸ Mutumiki anabwela kuli Jehu, kukamba kuti, "Baleta mitu za bana bamuna ba mfumu." Chakuti anakamba kuti, "Yaunjikeni pabili gate paka kuseni." ⁹ Kuseni Jehu anayenda panja naku imilila, naku kamba kubantu bonse, "ndimwe osalakwa onani napangila mbuye wanga chiwembu naku mupaya, koma ni ndani anapaya bonse aba?" ¹⁰ Manje mufunika kuziba kuti palibe gawo ya mau ya Yahwe, mau yamene anakamba pa banja ya Ahab, yazagwa pansi, chifukwa Yahwe acita zamene anakamba kupitila mu mutumiki wake Elijah." ¹¹ Mwaicho Jehu anapaya bonse banasala mubanja ya Ahab mu Jezree, na bonse bamuna bofunika, bazake bapa fupi, naba nsembe bake, mpaka kulibe anasalapo pali beve. ¹² Ndipo Jehu anaimilila nakuyenda, anayenda ku Samaria. Pamene enze kufika pa Beth Eked ya mubusa, ¹³ anan kumana na akalongosi ba Ahazia mfumu ya Yuda. Jehu anakamba kuli beve, " Ndimwe ba ndani?" Banayanka, ndise baka longosi ba Ahazia, ndipo tiyenda pansi kuposha bana ba mfumu na bana ba mkazi wa mfumu Jezebel." ¹⁴ Jehu anakamba ku bamuna bake, " Batengeni ba moyo." Koteri anabatenga ba moyo nkau bapaya pangodi wa Beth Eked, bonse ba muna bali fote tuu. Sanasiyepo aliyense wamoyo pali beve. ¹⁵ Pamene Jehu ana chokako kuja, anakumana na Jehonadab mwana mwamuna wa Recab ku bwela ku kumana naye. Jehu ana muposha naku kamba kuli eve, " Mwati mtima wako uli naine, mwamene mtima wanga uli na wako?" Jehonadab anayanka, Ni mwanene." ¹⁶ Jehu anakamba, " Ngati vili soche, nipase kwanja yako." Koteri anapasa Jehu kwanja yake, ndipo Jehu anayenda na Jehonadab pa mwamba mu ma hosi. ¹⁷ Pamene anabwela mu samaria, Jehu ana paya bonse banasala m'mubado wa Ahab mu Samaria, mpaka na kuononga mzere za chifumu wa Ahab, monga mwamene bana bauza pasogolo pa mau ya Yahwe, yamene yana kamiwa kuli Elijah. ¹⁸ Pamenepo Yehu anasonkhanitsa anthu onse nanena nawo, Ahabu anatumikira Baala pang'ono, koma Yehu adzamtumikira kwambiri. ¹⁹ Tsopano itanani aneneri onse a Baala, olambira ake onse ndi ansembe ake onse. Munthu aliyense asasiyidwe, Ndasiya nsembe, chifukwa ndili ndi nsembe yayikulu yoperekera Baala. Aliyense amene sabwera sadzakhala ndi moyo. " Koma Yehu anachita izi mwachinyengo kuti aphe olambira a Baala. ²⁰ Yehu anati, "Khazikitsani nthawi yopangira Baala." Chifukwa chake adalengeza. ²¹ Kenako Yehu anatumiza uthenga mu Isiraeli yense, ndipo olambira onse a Baala anabwera, moti panalibe munthu aliyense amene sanabwere. Iwo analowa m templenyumba ya Baala ndipo inadzazidwa kuchokera kutsogolo mpaka kumbuyo. ²² Ndipo Yehu anati kwa wosunga m'chipinda chodyera cha wansembe, Tulutsa zovala kwa olambira onse a Baala. Natenepa mamuna aabweresa nguwo. ²³ Pamenepo Yehu anapita ndi Yehonadabu mwana wa Rekabu ku nyumba ya Baala, ndipo anati kwa olambira Baala, Funani, tsimikizani kuti pasapezeke mmodzi wa inu wochokera kwa atumiki a Yehova, koma olambira Baala okha. ²⁴ Kenako analowa kukapereka nsembe zopsereza. Tsopano Yehu anasankha amuna 80 amene anali atayimirira panja, ndipo anati kwa iwo, "Munthu aliyense amene ndidzawapereka m'manja mwanu akapululumuka, aliyense amene adzalole kuti munthuyo apulumuke, moyo wake udzapululumutsidwa ndi moyo wa amene wapulumukayo." ²⁵ Ndipo atangomaliza kupereka nsembe yopserezayo, Yehu anati kwa mlonda ndi kwa akapitao, Lowani, muwaphe; asatuluke aliyense. Pamenepo anawapha ndi lupanga, ndipo alonda ndi akapitawo anawaponya kunja, nalowa m'chipinda chamkati cha nyumba ya Baala. ²⁶ Iwo anakoka zipilala zamwala zimene zinali m'nyumba ya Baala, ndipo anazitentha. Ndipo anaphwanya chipilala cha Baala, ²⁷ nawononga nyumba ya Baala, naipanganso chimbudzi, kufikira lero. ²⁸ Umu ndi mmene Yehu anawonongera kupembedza Baala mu Israeli. ²⁹ Koma Yehu sanasiye machimo a Yerobowamu mwana wa Nebati, amene anachimwitsa nawo Israeli, ndiko kulambira ana a ng'ombe agolide a ku Beteli ndi ku Dani. Pamenepo ³⁰ Yehova anati kwa Yehu, "Popeza wachita bwino mwa

kuchita zoyenera pamaso panga, ndipo wachitira nyumba ya Ahabu monga mwa zonse zinali muntima mwanga, mbewu zako zidzakhala pampando wachifumu wa Israyeli kufikira mwana wachinayi. m'badwo. " ³¹ Koma Yehu sanasamale kuyenda m'malamulo a Yehova Mulungu wa Israyeli ndi mtima wake wonse. Sanasiye machimo a Yerobowamu, amene anachimwitsa nawo Israeli. ³² Ndipo m'masiku amenewo Yehova anayamba kudula zigawo za Israyeli; Hazaeli nakantha Aisrayeli m'malire a Israyeli, ³³ kuyambira Yordano kum'mawa, dziko lonse la Gileadi, ndi Agadi, ndi Arubeni, ndi Manase, kuchokera ku Aroeri, ndiwo ku chigwa cha Arinoni, kupyola ku Gileadi kufikira ku Basana. ³⁴ Nkhani zina zokhudza Yehu, zonse zimene anachita, ndi mphamvu zake zonse, zinalembedwa m'buku la zochitika za mafumu a Isiraeli. ³⁵ Yehu anamwalira ndipo anayikidwa m ancestorsmanda ku Samariya. Kenako Yehoahazi mwana wake anayamba kulamulira m'malo mwake. ³⁶ Nthawi yomwe Yehu analamulira Israeli mu Samariya anali zaka 28.

Chapter 11

¹ Manje pamene Atalia, mai wa Azalia, anaona mwana wake mwamuna anafa, anauka nakupaya bonse bantu baku nyumba ya mfumu. ² Koma Johoseba, mwana mkazi wa mfumu Jehoram na mulongosi wake Ahazia, anatenga Joash mwana wa Ahazia, naku mubisa kumuchosa pabana ba mfumu bamuna bame bana paiwa, na bonse bomusunga; anabaika mogona. ³ Anamubisa kwa Atalia kuti asapaiwe. Anankala naye kwa zaka sikisi, obisama mu nyumba ya Yehova, pamene Atalia anali kulamulila mumalo yaja. ⁴ ⁶ Muchaka cha seveni, Jehoiada anatuma uthenga na kubwelesa asilikali akulu akulu bali hundiledi baku Karatise nao londa, nakubaleta kuli eve, mapephelo mwa Yehova. Anapanga cipangano nabeve, anabauza kuti balapile mu nyumba ya Yehova, ndipo anabaonesa bana ba mfumu ba muna. ⁵ Anabalamulila nakubauza, "Ivi ndiye vamene mufunika kuika bo kwana batatu mubweler pa sabata muzankhala mulonda nyumba ya mfumu. Ndipo na bamenango batatu mubwele pa colobela, na benango bali batatu kumbuyo kwa nyumba naku cingiliza." ⁷ Ma gulu ena yabili yamene siyatumikila pa sabata, mulonde nyumba ya Yehova ya mfumu. ⁸ Mfunukuila kuzungulilira mfumu, mwamuna aliyesense na cida cake mumanja. Aliyense amene aloba pa ukulu wanu, apaiwe. Munkale na mfumu pamene iyenda kunja, napamene iloba. ⁹ Mkulu wa nkondo anamvela vonse vamene anabalamulila wa sembe Jehoida. Aliyense atenga amuna bake, banja bamene sibili kutumikila pa sabata, na baja bamene bali kuleka kutumikila pa sabata; bana bwela kwa Jehoida wa sembe. ¹⁰ Koma Jehoida wa sembe analamulira mazana amikono na mikondo za Davide nazonse zinali mu nyumba ya Yehova. ¹¹ Ndipo otumikila, mwamuna aliyense na cipangizo cake mumanja, ku manja yamanja ya mopekelela naku manzele, pafupi na guwa na mopepelela, kuzungulila mfumu. ¹² Pamene apo Jehoida wa sembe analeta bana ba mfumu Joash, amunaika cisote caumfumu pali eve, ndipo anamupanga mfumu nakumuzozan eve. Bana tota mumanja nakukamba kuti, "Mfumu munkale muyaya." ¹³ Pamene Atalia anamvela chongo ca olonda na bantu, anabwela kuli bantu mu tempele ya Yehova. ¹⁴ Anayangana, ndipo, ana ona kuti, mfumu yaimilila pa choimilila, monga mwa cikhalidwe chao cinali, asogoleri na oliza lipenga anali na mfumu. Bantu bonse bamu maiko yaja anali okodwa ndipo analiza malipenga. Ndipo Atalia anang'amba vomvala vake naku punda mokuwa, "milandu milandu!" ¹⁵ Ndipo Jehoiada wa sembe analamulira akulu akulu ba bantu bambili bankhondo, nakukamba, "mubweleseni pa mpanda. Aliyese wamene amukonka, mupayeni na lupanga." Chifukwa wa sembe akamba, "Musalole kuti apaiwile mu nyumba ya Yehova." ¹⁶ Anamuleka pamene analikufika pafupi na malo pamene akavalo aloba mu'malo amfumu, ndipo anapaiwa. ¹⁷ Ndipo Jehoiada anapanga chipangano pakati pa iye na Yehova na mfumu na banthu. Kuti bankhale banthu ba yehova, ndiponso pa banthu na mfumu. ¹⁸ Ndipo banthu mu malo banayenda ku nyumba ya Baala nakuononga. Banapaya mattani, wa sembe wa Baala pa guwa onse aiona. Ndipo Jehoiada wa sembe anasankha olonda nyumba ya Yehova. ¹⁹ Jehoiada anatenga olamulira akulu ona banthu mahandiledi, ndi onse na otumikila, nabanthu bonse bamuchalo baja, onse banaleta mfumu pansi coka ku nyumba ya Yehova anayenda ku nyumba, kuloba pa colobela ca otumikila. Joash anatenga malo yake ya umfumu. ²⁰ Anthu onse amu malo yaja anakodwa, malo yanalibe chongo pamene Athalia anapaiwa ku nyumba ya mfumu. ²¹ Joash anali nazaka seveni pamene anayamba kulamulila.

Chapter 12

¹ Mu chaka cha nambala 7 cha Jehu, kulamulila Joashi kunayamba analamulila zaka fote mu Yelusalemu. Amai bake zina anali Zibiah, waku Beersheba. ² Joashi anachita voyenela pamaso pa Yehova ntawi zonse, chifukwa Yehoiada wa nsembe anamuza kuata iye. ³ Koma malo ya anasmbe sanate ngedwe. Banthu banapitiza kuyereka nsembe izo shoka nazo nunkhula pa malo ya pa mwamba. ⁴ Joashi anati kwa ansembe, "Ndalama zonse zamene zipereke ngati choyera chopereka mu nyumba ya Yheova, ndalama izo aliyense ayesedwe-ngati ni ⁵ Wansembe aalandile zopereka zonse kuchoke, a ku bantu osunga ndalama kuti apange futi zonse zo-onogeka mu nyumba ya Mulungu. ⁶ Koma pakati pa zaka 23 chaka cha ulamulilo wa Joash, wa sembe ali kukonza zoonongeka ma tempere. Mfumu Joash anaitana Jehoiada wa sembe na benengo asembe; nakamba kuli beve " Nichifukwa chani simunakonze mu nyumba ya Mulungu? ⁷ Manje musatenge ndalama iliyonse kwa osonkhesa, koma tengani zamene zatengewa kudala zokozela tempere zipaseni kuli awoamene afunika kukoza kachisi." ⁸ Asembe anakana kutenga ndalama zili zonse kuchokela ku banthu na kuti basakonze malo opephelela beve beka. ⁹ Mumalo mwakuti, Jehoiada wa sembe anatenga cifuba chake, cholasila chake na chovalira, nakuchiika pafupi na guwa kun mbali ya liiti pamene wina angana mu nyumba ya Yehova. Asembe amene anali kulonda tempere polobela nakuika pamodzi ndalama zonse zamene zina bwelesewa mu nyumba ya Yehova. ¹⁰ Pamene banaona kuti muli ndalama zambili mucosungilamo, mfumu ya sudukju na wa sembe mkulu anali kubwela nakuika ndalama zopezeke mu tempere ya Yehova. ¹¹ Bana pasa ndalama zamene zinaong'e'a mamapya ya banthu bamene banali kusunga tempere ya Yehova. Banapasa bopala matabwa (okonza mipando) na omanga manyumba, amene anali ku konza nyumba ya Yehova, ¹² ndipo kwa amasoni na ojuba miyala naku konza tempere ya Yehova, na zonse zimene zizofunika kupasiwa kuti akonze. ¹³ Koma ndalama zobwelesewa mu nyumba ya Yehova sizinaperekewe kuti apange kapu ya siliva, hoimbilako liti, kabata, lipenga, kapena golidi kapena sliva yoonesela bwino. ¹⁴ Banapasa ndalama ii kwa bonse bamene bana guwira nhito mu nyu nyumba ya Yehova. ¹⁵ Kuonjelapo, sibanafune ndalama kuibelengelako amene inapasiwa ba nchito ba muna, chifukwa anthu aba benze bonkhulupilika. ¹⁶ Koma ndalama zopereka chifukwa ca machimo na ndalama ya chimo yopereka sizinali kubwelesewa mu nyumba ya Yehova, Chifukwa zinali za asembe. ¹⁷ Hazeal mfumu ya Aram anamenya naku paya a Gathi, nakutenga icho. Hazeal anabwela nakumenya Yerusalemu. ¹⁸ Joash mfumu ya Ayuda anatenga zinthu zonse zamene Jehoshaphat na Jehoram na Ahaziah, atate bake, mfumu ya Yuda, nakuika pa tela, na golide yonse imene inapezeke mosungilamwa nyumba ya Yehova na mfumu inatuma Hazziel mfumu ya Aran, Ndipo Haziel anachoka ku Yerusalemu. ¹⁹ Koma kwa nkani zina zamene pa Joash, zimene anacita niku, sizinaembewe mu buku ya zocitika mu mafumu ya Yuda. ²⁰ Anchito bake anaukira pamodzi, naku menya Joash mu Beth Millo, yamene igandelela kufika ku Silla. ²¹ Jozabad mwana wa Shimeath, na Jehozabad mwana wa Shomer, wa nchito wake, anamumenya eve, anafa. Anamuika mumanda, Joash na makolo ake akudala mu malo ya Davide, na Amaziah, namwana waka mwamuna, anankala mfumu mu nyumba yake.

Chapter 13

¹ Caka ca twenti-fili cha Joash mwana wa Ahaziah mfumu ya Yuda, Jehoahaz mwana wa Jehu anayamba kulamulila Israyeli Samaria; analamulira zaka seventini. ² Anacita cinthu chamene cinali choipa pa menso ya Yehova na kukonkha machimo ya Jeroboam mwana mwamuna wa Nebat, analenga Israyeli kuchimwa; Jehoahaz sanacoke kwa beve. ³ Ukali wa Yehova unashoka Israyeli, anapitiliza kubapasa mu manje ya Hazael mfumu ya Aram na mmanja ya Ben Hadad mwana mwamuna wa Hazael. Koma ⁴ Jehoahaz ana pempha Yehova, na Yehova anamvela kwa eve chifukwa anaona kumuutsira kwa bana ba Israyeli, mwamene mfumu ya Aram inababvutisira beve. ⁵ Ndipo Yehova anabapulumusa bana ba Israyeli, bana pulumuka mu manja ya Arameans, na banthu ba Israyeli banayamba kunkhula mu manyumba yao monga kudala. ⁶ Komatu, sibanacokeko machimo ya nyumba ya Jeroboam, amene analengesa Israyeli ku cimwa, anapitiliza mu macimo ayo; na kupitiliza na fano mu Samaria. ⁷ Aramean anamusiya Jehoahaz na banthu bapa kavalo bali fifite, naboyenda pansi bali teni sauzandi, na akavalo teni ya mfumu yaku Aram anaononga anabapanga monga dothi yopodelapo. ⁸ Pankani zina zija Jehoahaz, anacita na mphamvu, kodi sivalenbewe mu mabuku ya zocitika mu mfumu ya Israyeli? ⁹ Ndipo Jehoahaz anagona na makolo ake, ndipo bana muika ku Samaria. Jehoash anankhala mfumu ku malo kuja. ¹⁰ Mu caka ca theti-seveni Joash mfumu ya Yuda, ulamuliro wa Jehoahaz unayamba mu Samaria na mu Israyeli; analamulira zaka sikisitini. ¹¹ Anacita coipa ku Yehova. Sana siye macimo ya Jeroboam mwana mwamuna wa Nebat, mwa ichi anapanga Israyeli kucimwa, koma anayenda muli eve. ¹² Vocita vinango va Jehoash, na vonse vamene anacita, mwa mphamvu yake kuti anamenya Amaziah mfumu ya Yuda, kodi sivalenbewe mu buku ya vocitika mfumu ya Israyeli? ¹³ Jehoash anagona na makolo ake akudala, na Jeroboam anakhala pa mpando wa cifumu. Jehoash anakwa mumanda mu Samaria na mfumu yaku Israyeli. ¹⁴ ¹⁵ ¹⁶ Manje Elisha anabwela adwala mateda ndipo anabwela afa, amufikira Jehoash mfumu ya Israyeli nakulira kuli iye. Anati, "Atate banga, atate banga, gareta wa Israyeli na akavalo na banthu bake batengewa kuli iwe!" Elisha anati kulin eve, "Tenga uta na colasila," Ndipo Joash anatenga uta na volasila. Elisha anakamba kuli mfumu ya Israyeli Kuti, "Ika manja yako pa muvi," Anaika kwanja yake pa ichi. Elisha anaika kwanja yake pa manja ya mfumu. ¹⁷ Elisha anati, "Bvula ma windo yaku m'mawa," ndipo anayasegula. Pamenepo Elisha anakamba kuti, "Mulase!", Ndipo ana mulasa. Elisha anati, "Uyu ni mukondo wa Yehova wa ciaonjeco, mkundo woganyesera Aramu, kuli iwe uzamenya ba Aramean mpheke mpaka ubasilize bonse. ¹⁸ Ndipo Elisha anakamba kuti, "Tenga ka mkondo," Joash anatenga. Anati kuli mfumu ya Israyeli, "Menya pansi na yeve," na menya katatu pansi, naleka. ¹⁹ Koma munthu wa Mulungu anakalipa kwambili na eve anakmba, "Sembe unamenya pansikali faive kapena kali sikisi. Sembe wa menya ba Aram mpaka wa basiliza, koma manje uzamenya Aram kali katatu." ²⁰ Ndipo Elisha anafa, anamuika kwamene kuja. Ndipo gulu ya Moab inatenga malo ya kuyamba kwa caka. ²¹ Pamene bakali kuika munthu wina, banaona gulu ya a Moab, banataya thupi ya munthu uja mu manda ya Elisha. Pamenepo munthu uja wakufa anakumiya maboza ya Elisha, anauka nakuimilira futi. ²² Hazael mfumu ya Aramu anabvutisa ba Israyeli masiku yonse ya Jehoahaz. ²³ Koma Yehova anali anakondo ba Israyeli, anabactilira cifundo ba kwambili, cifukwa ca pangano pakati pa iye na Abrahamu, Isaki, na Yakobo. Manje Yehova sana ba ononge beve, sana chose pa menso pake. ²⁴ Hazael mfumu ya Aram anafa, ndipo Ben Hadad mwana wake anaikiwa mfumu mumalo mwake. ²⁵ Jehoash mwana wa Jehoahaz anatenga cosa kwa Ben Hadad mwana wa Hazeal malo yamene yanatengedwa kucosa kwa Jehoahaz na Atate ake mwa nkondo. Jehoash anamenya iye katatu, anatenga futi malo yonse ya Israteli.

Chapter 14

¹ Mucaka cacibili ca Jehoash mwana wa Jehoahaz, mfumu ya Israyeli, Amaziah mwana wa Joash, mfumu ya Yuda, anayamba kulamulira. ² Anali wazaka twenti-faivi pamene anayamba kulamulira; analamulira kwa zaka twenti-naine mu Yerusalemu. Amai ake zina anali Jehoaddad, waku Yerusalemu. ³ Anacita zabwino pameso pa Yaweh, koma sanali monga atate bake Davide. Anacita zonse zomwe Joash, atate ake anacita. ⁴ Koma malo yapamwamba siyanatengedwe. Banthu banapitiliza kuereka sembe ana shoka pamwamba paja. ⁵ Zinali pamene kulamulira kwake kumunkhazikisiwa, anapaya wa nchito amene anapanga atate bake mfumu. ⁶ Manje sanafune kupaya mwana waya wopanga kuti Atteli; koma, malo mwake, anacita monga vinalembewa mu buku ya malamulo ya Mose, monga Yaweh analamulira kuti, " Atate asapayewe cifukwa ca banabawo, kapena bana kupaiwa cifukwa ca macimo ya makolo yawo. Malo mwake, aliyense pawine cifukwa ca macimi yake." ⁷ Anapaya masauzandi ten ya asilikali baku Edom ku ku cigwa ca Salt; anatenga Sela mu nkondo naikuipasa zina kuti Joktheel, ndiye mwamene ikambiliwa nalelo. ⁸ Pamenepo Amaziah anatuma banthu bake kuli Jehoash mwana wa Jehoahaz mfumu ya Israyeli, anati, " Bwelani tikumane menso na menso mu nkondo." ⁹ Koma Joash mfumu ya Israyeli anatuma banthu bake kuli Amaziah mfumu ya Yuda, nakuti, " Ine ame utumikila ku Lebanon kuti atuma uthenga kuli mkunguza waku Lebanon, nakuti, ' Mpase mwana wako mukazi kuli mwana wanga mwamuna ankale mukazi wake; koma cinyama cofoya caku Lebanon iliti kuyeela moteyela naku dyaka pa colila. ¹⁰ Watimenya zoonza kuno ku Edom na mtima wako wakungamula pamwamba, iwe na Yuda na iwe?" ¹¹ Amaziah sanamvelele. Motero Jehoash mfumu ya Israyeli anamenya Amaziah mfumu ya Yuda anakumana menso na menso ku Beth Shemesh, malo ya Yuda. ¹² Yuda anali anagonjesewa anayenda ku nyumba kwao. ¹³ Joash mfumu ya Israyeli, anagwira Amaziah, mfumu ya Yuda mwana wa Jehoash Ahaziah, ku Beth Shemesh. Anabwela ku Yerusalemu kuononga vomanga vaku Yerusalemu kucokela ku cipata kuli Ephramu cipata kung'ono kuja, za mikono handiredi anali kulipha kwake. ¹⁴ Anatenga golide na siliva yonse, na zinthu zonse zinali mu nyumba ya Yahwe, vinthu vonse va mtengo wapamwamba vamu nyumba ya mfumu, nabo ongwiliwa onse, ndipo banabwelerana ku Samaria. ¹⁵ Kwa macitidwe ena onena pa Joash, zonse anacita, mphamvu yake, namwamene anamenyerana na Amaziah mfumu ya Yuda, sizinalembedwe mu buku ya zocitika za mfumu ya Israyeli? ¹⁶ Ndipo pamenepo Joash anagona na makolo ake chokonkhao ana ikiwa mu Samaria na mfumu ya Israyeli, na Jeroboam, mwana wake, mankhala mfumu munalo mwake. ¹⁷ Amaziah mwana wa Joash, mfumu ya Yuda, anankala zaka fiftini pambuyo yaifa ya Jehoash mwana wa Jehoahaz, mfumu ya Israyeli. ¹⁸ Monga mwa manje pankhani zokamba Amaziah, kodi sizinalembedwe mu buku ya zocitika za mfumu ya Yuda? ¹⁹ Anapangira ciwembu Amaziah mu Yerusalemu, na yanda ku Lachish, koma anatuma banthu ku Lachish na kumupaya kwamene kuja. ²⁰ Boma muleta pa kavelo, anaikiwa na makolo ake mu malo ya Davide. ²¹ Banthu bonse ba Yuda anatenga Azariah, amene anali zaka sikisitini, nakupanga mfumu mumalo mwa atate bake Amaziah. ²² Anali Azariah anamnga Elath ndipo ansbweza kwa Yuda, mfumu iyi inaikiwa na makolo aka. ²³ Mu caka ca fiftini ca Amaziah mwana wa Joash mfumu ya Yuda, Jeroboam mwana wa Jehoash mfumu ya Israyeli anayamba kulamulira ku Samaria; analamulira kwa zaka fote-wanu. ²⁴ Anacita chamene cinali coipa pa menso ya Yahwe. Sanacoke ku macimo ya Jeroboam mwana wa Nebat, amene analengesa Israyeli kucimwa. ²⁵ Anabwezela ku malile ya Israyeli kucokela ku Lebo Hamath mpaka ku manzi ku Arabah, kukonkha kulamulira kwa Yahwe, Mulungu wa Israyeli, anakambapo kwa anchito a Jonah mwana wa Amittai, muneneli, amene anali kuchokera ku Gath Hepher. ²⁶ Pakuti Yahwe anaona kubvutika kwa bana ba Israyeli, cinali cobaba kwa aliyese, bonse akapolo na bosamangiwa, nakuti kunalibe obapulumusa bana ba Israyeli. ²⁷ Potero Yahwe anati sazaononga zina la Israyeli pansi pa kumwamba; koma, anabapulumusa na kwanja yakwa Jeroboam mwana wa Jehoash. ²⁸ Koma pa nkhanu zina zobvutika zonena pali Jeroboam, pazonse anacita, anacita nkondo naku tenga Damascus na Hamath, yamene yanali ya Yuda, za Israyeli, kodi sizinalembewe mu buku ya zocitika za mfumu ya Israyeli? ²⁹ Jeroboam anagona na makolo ake na mfumu za Israyeli, na Zakaria mwana wa mfumu mumalo mwake.

Chapter 15

¹ Mu caka ca twenti-seveni Jeroboam mfumu ya Israyeli, Azariah mwana wa Amaziah mfumu ya Yuda anayamba kulamulira. ² Azariah anali na zaka sikisitini pamene anayamba kulamulira, kwa zaka fiftite-tu mu Yerusalemu. Amai ake zina yabo banali Jekoliah, anali aku Jerusalem. ³ Anacita zoyera pamene Yahwe munga atate bake banacitilira. ⁴ Zinali pamene, malo ya pamwamba siyanatengewe. Banthu banali bakali kupeleka nsembe na kushoka zonukhila pamalo ya pamwamba. Yehwe anaidwalitsa mfumu kuti inankhala na khate mpaka siku ya kufa anakhala mu nyumba inango. ⁵ Yotamu, mwana wa mfumu anali mu nyumba muja ndipo analamulira mu malo muja. ⁶ Koma nkhanzi zinango zokamba pali Azariah, zonse zamene anacita, sizinali zinalembewa mu buku ya zo itika ya mfumu ya Yuda? ⁷ Choncho Azariah anagona na makolo ake akudala; anaikiwa na makolo bake mu malo ya Davide. Yotamu, mwana wake, anabwela ankhala mfumu mu malo muja. ⁸ Mu caka ca feti-eyitica Azariah mfumu ya Yuda, Zakariya mwana wa Jeroboam analamulira mu Israyeli mu Samaria kwa miyezi sikisi. ⁹ Anacita camene cinali coipa pa menso ya Yahwe, munga atate bake banacita. Sana leke kuli aytate bake Jeroboam mwana wa Nebat, Analengesa Israyeli kuchimwa. ¹⁰ Shallum mwana wa Jabesh banayenga Zakariya, banamumenya ku Iblem, nakumupaya, Ndipo anakhala mfumu eve mumalo yaja. ¹¹ Kukamba pa nkhanzi zokamba pali Zakariya, zinalembewa mubuku ya zocitika mu ufumu wa Israyeli. ¹² Aya yenze mau ya Yahwe kuti anakmba na Jehu, nati," Makolo yazankhala pa mupando wa ufumu mu mibado wa ufumu ili foo ibwela." Izi ndiye zinacitika. ¹³ Shallum mwana wa Jabesh anayamba kulamulira mu caka ca fetini ca Azariah mfumu ya Yuda, ndipo analamulira cabe mwezi unozi mu Samaria. ¹⁴ Menahem mwana wa Gadi anayenda ku Tirzah nakufika ku Samaria. Anamenya Shallum mwana wa Jabesh, mu Samaria. Anamupunga nakunkhala mfumu mu malo yaja. ¹⁵ Kukamba pankhani zina zokamba za Shallum na ciwembu anapanga, zinalembewa mubuku yazocitika mubuku ya mafumu ya Israyeli. Pamenepo ¹⁶ Menahem anacitira ciwembu Tipsah na onse anali pamenepo, na malire yaku Tirzah, cifukwa sibanasegule malo kuli eve. Ndipo anamenya icho, anatumula bakazi bonse bamamimba mu munzi uja. ¹⁷ Caka ca feti-naini ca Azariah mfumu ya Yuda, Menahem mwana wa Gadi anayamba kulamulira Israyeli; analamulira kwa zaka teni mi Samaria. ¹⁸ Anacita coipa pamenso pa Yahwe. Mumoyo wake wonse, sana coke ku macimo ya Jeroboam mwana wa Nebat, amene analengesa Israyeli kucimwa. ¹⁹ Pamenepo Pul mfumu ya Assyria anabwela kumenyana a calo, na Menahem anapasa Pul wanu sauzande matalanta ya siliva, kuti Pul manja yake yankhale naye kupasa mphamvu ufumu wa Israyeli mu manje yake. ²⁰ Menahem anasonkhesa ndalama za cuma cao kuti apase masekeli fiftite asiliva kuti apase mfumu ya Assyria. Pamenepo mfumu ya Assyria anakana nabweza sanakhale mu malo muja. ²¹ Koma kukamba za Menahem, na vonse vamene acita, kodi sivina lembewe mubuku yazocitika mu mfumu ya Israyeli? ²² Sopano Manehem anagona na makolo yake, na Pekahiah mwana wake mwamuna anankhale mfumu. ²³ Mucaka ca fiftite ca Azariah mfumu ya Yuda, Pekahiah mwana mwamuna wa Menahem anayamba kulamulira Israyeli mu Samaria; analamulira zaka tuu cabe. ²⁴ Anacita coipa pamenso pa Yahwe. Sanasiye macimo ya atate bake Jeroboam mwana wa Nebat, mwaichi apanga Israyeli ku cimwa. ²⁵ Pekahiah anali na ofisa zina yake Pekah mwana wa Remaliah, amene anapanga ciwembu caiye. Na amuna bali fiftite baku Gileadi, Pekah anapaya Pekahiah na Agrob na Arieah mu Samaria, mu katedeo mu nyumba ya mfumu. Pekah anapaya Pekahiah nankhals mfumu mu malo mwake. ²⁶ Koma Kukamba pa nkhanzi zokamba pa za Pekahiah, zonse anacita, zinali zolembewa mubuku ya zocitika mu umfumu ya Israyeli. ²⁷ Caka ca fiftite-tuu ca Azariah mfumu ya Yuda, Pekah mwana wa Remaliah analowa mu ufumu wa Israyeli mu Samaria; analamulira zaka tuu. ²⁸ Anacita camene coipa pamenso ya Yahwe. Sanali anacoka koma cimo ya Jeroboam mwana wa Nebat, amene anapanga kuti Israyeli kucimwa, ²⁹ Mu masikuu ya Pekah mfumu ya Israyeli, Tiglath-Pileser mfumu ya Assyria anabwela nakutenga Ijon, Abel Beth MMAacah, Janoah, Kedesh, Hazor, Gilead, Galilee, na calo conse ca Naphtali. Anabatenga kupita nao ku Assyria. ³¹ Ndipo Hoshea mwana mwamuna wa Elah anapanga ciwembu kuli Pekah mwana mwamuna wa Remaliah. Anamumenya nakunupaya iye. Anabwela ankhala mfumu mu nyumba ya mfumu mu caka ca twente ca Yotamu mwana mwamuna wa Uziah. ³⁰ Pali nkhanzi zina za zonena pali Pekah, zonse zamene anacita, zinalembewa mubuku yazocitika mu ufumu wa Israyeli. ³² Mu caka ca tuu ca Pekah mwana mwamuna wa Remaliah, mfumu ya Israyeli, Yotamu mwana mwamuna wa Azariah, mfumu ya Yuda anayamba kulamulira. ³³ Anali na zaka twenti-faivi pamene anayamba kulamulira; analamulira cabe zaka sikisitini mu Yerusalemu. Amai ake zina anali Jerushah; anali mwana mukazi wa Zadok. ³⁴ Yotamu anacita zabwino pamenso ya Yahwe. Anakokha cisanzo ca atate bake Azariah anacita. ³⁵ Komatu, malo yapamwamba siyanatengewe. Banthu bali kupereka nsembe zoshoka pamwamba Yotamu anamanga cipata cakumwamba ca nyumba ya Yahwe. ³⁶ Koma pa nkhanzi zina zokamba pa Yotamu, na zonse zinalembewa mubuku ya zocitika mu umfumu wa Yuda. ³⁷ Mu masiku ayo Yahwe anayamba kutuma bomenyana na Yuda Rezim mfumu ya Aram, na Pekah mwana mwamuna wa Remaliah. ³⁸ Yotamu

anagona na makolo ake anaikiwa pamonzi mu malo ya Davide, makolo ake bakudala. Pamene apo Ahaz, mwana mwamuna wake, anankhala mfumu mumalo mwake.

Chapter 16

¹ Mu caka ca seventini ca Pekah mwana mwamuna wa Remaliah, Ahaz mwana mwamuna wa Yotamu mfumu ya Yuda, anayamba kulamulira. ² Ahaz anali ndi zaka twentipamene anayamba kulamulira, analamulira zaka skisitini mu Yerusalemu. Sanacite coyenera pamenso pa Yahwe Mulungun wake, monga mwamene makolo ake Davide anacitira. ³ Koma, anayenda monga mafumu ya Israyeli; zoona, anapanga kuti mwana wake apite mu mulilo, kukonkha voyesa vocitika mucalo, zimene Yahwe anacosa pamenso ya Israyeli. ⁴ Anapereka nsembe zoshoka zonunkhila pamwamba, pansi pa zobilibila pamtengo. ⁵ Ndipo Rezin, mfumu ya Aram na Pekah mwana mwamuna wa Remaliah, mfumu ya Israyeli, anabwela ku Yerusalemu mukumenya. Bana mulepesa Ahaz, koma sibanamukngonjese iye. ⁶ Pa nthawi iyo, Rezin mfumu of Aram anabwezela Elath kuli Aram na kucosa amuna ba Yuda mu Elath. Ndipo Arameans anabwela ku Elath kwamene banankhala mpaka lelo. ⁷ Pamene apa Ahaz anatuma opereka uthenga ku Tiglath-Pileser mfumu yaku Assyria, nakuti, "Ndine wa nchito wako na mwana wako. Bwela kuno unipulumuse mu manja ya mfumu yaku Israyeli bamene banimenyana ine." ⁸ Koma Ahaz anatenga siliva na golide zamene zinapezeka mu nyumba ya Yahwe na katundu yamene inali mu nyumba ya mfumu nakuzipela ngati mphaso ku mfumu yaku Assyria. ⁹ Mfumu yaku Assyria anamvelela eve, ndipo mfumu yaku Assyria inamenya Damascus, nakungonjese iyo nakukunyamula banthu bake kunkhala andende ku Kir. Anapayanso Rezin mfumu yaku Aram. ¹⁰ Mfumu Ahaz anayenda ku Damscus kuti akumane na Tiglath-Pileser mfumu ya Assyria. Ku Damascus anaona guwa. Anatuma Uriya wa nsembe amene alini cionekelako cake ca guwa cifanizo cake pa nchito yake yonse yofunika. ¹¹ Ndipo Uriya wa nsembe anamnga guwa kuti mkhale monga mfumu Ahaz anafunila anatuma ku Damascus. Anasiliza pamene mfumu Ahaz asanabwele kucoka ku Damascus. ¹² Pamene mfumu inabwela kucoka ku Damascus anaona guwa; mfumu inafika pafupi na guwa nakupasa copereka pa iyo. ¹³ Anapanga copereka na kupereka nsembe zo imiwa za ku munda copereka, anathira pa guwa cakumwa pa iyo ngati copereka, anawaza magazi ya kusankhana copereka pa guwa. ¹⁴ Guwa ya mkuwa yamene inali pa Yahwe-anaibwelesa pasogolo pa tempele, pakati pa guwa na tempele ya Yahwe nakuika ku mphoto kwa guwa. ¹⁵ Mfumu Ahaz analamulira Uriya wa nsembe, nakukamba kuti, "Paguwa ikulu shoka kuseni zoshoka zopereka na mumazulo zopereka zakumunda, zopereka zoshoka za mfumu na zopereka zoimila anthu onse ba mu mzinda uja, na zopereka zakumunda na zakumwa zoeleka. Thila momwaza magazi ya nsembe yoshoka na magazi yonse ya nsembe. Koma guwa ya mukwa izankhla yanga yofumisilaka moyendela." ¹⁶ Uriya wa nsembe annacita zamene mfumu Ahaz analamulira. ¹⁷ Mfumu Ahaz anacosa masekele zo amphaka nacosa mimo pa anasisa thawale: pamwamba pa ng'ombe zinali pansi pake nakuika pamwamba miala. ¹⁸ Anacosa cobisa capa sabata camene banamanga pa nyumba ya Mulungu, pamozi na mfumu pongenera kunja kwa nyumba ya Yahwe, cifukwa ca mfumu ya Assyria. ¹⁹ Pa nkhani zinango zokamba pa Ahaz na zamene anacita, kodi sizinalembewe mubuku ya zocitika mu mfumu wa Yuda? ²⁰ Ahaz anagona na makolo ake anaikiwa na makolo ake mumalo ya Davide. Hezekiah mwana mwamuna wake anabwela ankhala mfumu mu malo mwake.

Chapter 17

¹ Mu chaka twavu ca Ahaz mfumu ya Yuda, kulamulira kwa Hoshea mwana mwamuna wa Elah kunayamba. Analamulira Samaria pa Israyeli kwa zaka naine. ² Anacita chamene chinali coipa pamenso pa Yahwe, koma osati mfumu ya Israyeli amene analipo kudala pamene iye asankhalepo. ³ Shalmaneser mfumu ya Assyria, anamenya iye, na Hoshea anakhala wa nchito wake nakumupasa mutulo. ⁴ Ndipo mfumu ya Assyria anaziba kuti Hoshea afuna kumenya nkondo eve, Hoshea anatuma amthenga ake kuli mfumu yaku Egypto; na, azipeleka kupasa kwa mfumu ya Assyria, monga anacita caka na caka. Koma mfumu ya Assyria anamulesa kukamba naku mumanga, nakumuika mujele. ⁵ Ndipo mfumu ya Assyria anamenya bamu malo yaja bonse nthawi yonse, nakumenya Samaria nakumangira mwa zaka firi. ⁶ Mu caka ca naiane ca Hoshea. mfumu ya Assyria anatenga Samaria nakutenga Israyeli kuyenda nayo ku Assyria. Anabaika mu Halah, pambali pa kamana ka Gozan, na mumalo ya Medes. ⁷ Kumangiwa uku kunacitika cifukwa chakuti Israyeli anali ana cimwa pamenso ya Yahwe mulungu wao, wamene anabachossa ku malo ya Egypto, kucoka mumanja ya Farao, mfumu yaku Egypto. Banthu aba banali kupempela tumilungu twinago ⁸ nakuyenda mu miyambo ya chalo chamene Yahwe wao anabacosamo banthu ba Israyeli, mwakucita kwa mfumu ya Israyeli kuti banacita. ⁹ Banthu ba Israyeli bacita mwakabisila-nafuti Yahwe Mulungu wao-vinthu sivali voyenela. Banamanga beka malo yapamwamba mumalo muja, kucoka nsanja yolonda. kwamene kwamene kuli munzi kwamene uko. ¹⁰ Banaika voimila va milala vifanizo pa citunda ciliconse citali na pamtengo yonse kufika ku lupili. ¹¹ Apo banashoka zonukhilisa monse mu malo yapamwamba, monga calo cinali ku citita, baja bamene Yahwe anatenga kuli eve. Bana ba Israyeli bana cita voipa pamenso pa Yahwe. Vamene vinakalipisa Yahwe kuti akalipe; ¹² bana pempela mafano, zimene Yahwe anakamba nao beve, "Simuzacita izi zinthu." ¹³ Koma Yahwe anacita umboni pali ba Israyeli na Yuda mwan mneneri aliyense ananena, "Cokani ku macimo yanu sungani malamulo na malemba yanga, muikelo nzeru kusunga malamulon yanga yonse kusunga yamene nina lamulira atate banu, na yamene natuma kwa inu." ¹⁴ Koma sibanamvelele; bana yumisa mikosi yao monga azitate bamene sibana khulupilire muli Yahwe Mulungu wao. ¹⁵ Banakana malemba yake na cipangano camene analambila nakubapasa beve. Banakokha zocitika zacabe na beve bankhala ba cabe c abe. Banakokha calo cha banthu bosapemphele. bamene bezeli pakati pao, bamene Yahwe anakamba kuti musabakokhelele. ¹⁶ Bana siya malamulo yonse ya Yahwe Mulungu wao. Banapanga zopanga zbili za bana bang'ombe zibili kuti apembeze cifanizo bacipembeza banapembeza nyenyezi zonse na Baal. ¹⁷ Bana panga bana bao amuna na bakazi kupita pa mulilo. Banao ombeza nakucita va nyanga, banazimgulisa beka nakucita coipa pamenso pa Yahwe, bana mukalipisa anakalipa. ¹⁸ Ndipo Yahwe anakalipa manigi na Israyeli nakubacosa beve pamenso pake. Kuli anasal koma cabe Yuda eka. ¹⁹ Naeve Yuda sana sunge malamulo ya Yahwe Mulungu wao, bana konkha zocita zamene Israyeli anacitapo. ²⁰ Choncho Yahwe anakana mibado ya Israyeli; anaba nzunza nakupasa monga kwa awo bamene banga ononge, kufikila abacosa pamenso pake. ²¹ Anacosa Israyeli ku banja ya ufumu wa Davide, nakupanga Jeroboam mwana mwamuna wa Nebat mfumu. Jeroboam anacosa Israyeli kutali kukonkha Yahwe nakubanga cimwe. ²² Banthu ba Israyeli anakokha macimo ya Jeroboam anacosa ndipo sibana cokeko kuli ivo, ²³ Ndipo Yahwe anacosa Israyeli pamaso pake, monga anakambila mwa atumiki bake kuti azacita. Israyeli anapishiwa pa malo yawo na Assyria, Ndipo zikali sochabe nalelo. ²⁴ Mfumu ya Assyria analeta banthu baku Babylon na baku Kuthah, na baku Avva, na baku Hamath na baku Sepharvaim, nakubaika mu malo yaku Samaria malo yamene yanali ya Israyeli. Bantenga malo aya nakunkhalapo beve ku Samria. ²⁵ Zinacitika pamene banayamba kukhala kuti sibanalemekeze Yahwe. Ndipo Yahwe anatuma mikango yamene inapaya banthu benango. ²⁶ Banakamba na mfumu ya Assyria, nakukamba, "Calo camene mwatenga na ciika mu Samaria simuziba zocita zabanthu ba mucalo icho. Anabatumula mikango ipaya banthu kuja cifukwa sibanacite zamene Mulungu wa calo cija afuna. ²⁷ Mfumu ya Assyria inalamula, kuti, "Tengani wa nsembe umozi namene munabwelesa kucoka kuja, mumulole ankhale kuja, mulekeni abaphunzise banthu zocita zamene mulungu wa calo cija afuna. ²⁸ Ndipo umozi wa ansembe wamene banaleta kucoka ku Samaria nakubwela kukhala mu Bethel; anabaphunzisa molemekezela Yahwe. ²⁹ Magulu yonse yanapnga milungu yao, nakuyaika pamwamba malo yamene ya Samaria anapanga mu magulu onse ali kunkhala. ³⁰ Banthu baku Babylon banapanga sucoti bemoti; nabanthu baku Kuthah banapnga Negral; na banthu baku Hamath banapnga Ashima; ³¹ na Avvites banapanga Nibhaz na Tarktak. Na Sepharvites bana shokabana bao pa muliro kuli ba Adrammelek na Anammelek, mulungu wa Sepharvites. ³² Banapasa ulemu Yahwe, banasankha umozi kunkhala wa nsembe wapa mwamba, anapereka nsembe zawo mu nyumba ya Mulungu pa mwamba pa malo. ³³ Anapasa ulemo Yahwe nakupembeza milungu yao, mu mwamba wa calo camene banatengewako, ³⁴ Nalelo banapitiliza na mwambo wakudala. Sabapasa ulemo Yahwe, kapena kunkamba malembo yake, zokamba zake, malamulo, kapena cilamulo cimene Yahwe anapasa abadwa bakwa Yakobo, amene anabapasa zina ya Israyeli. ³⁵

Pamene Yahwe anapanga pangano na beve, anabala mulira beve, " Musayope milungu inango, kapena kuigwadila iyo milungu, kapena kuipembeza, kapena kupereka nsembe kuli iyo. ³⁶ Koma Yahwe, anakailteni imwe kucoka ku malo yku Egypto na mphamvu yake na kwanja yake ya mphamvu, nikuli eve mufinika ku gwadila, nikuli eve mufunikala kuperekeka nsembe. ³⁷ Malemba na zokamba, malamulona cilamulo camene analembela imwe, musunge muyayaya. Musayope milungu inango, ³⁸ pangano yamene napanga naimwe, musaibale; ndipo musapase ulemu milungu inango. ³⁹ Koma Yahwe Mulungu wanu ndiye amene mufunikila kupasa ulemu. Azakakupulumusani imwe kuba ndani banu." ⁴⁰ Sibamvela cifukwa banapitiliza kucita zamene banali kucita kudala. ⁴¹ Koma maiko yonse banapsa ulemu Yahwe na kumupembeza na zosema, na bana ba bonse banacita izi-monga banacitila bana ba bana bao. Nalelo bakali kucita izi.

Chapter 18

¹ Ndipo munali mu caka ca citatu ca Hoshea mwana mwamuna wa Elah, mfumu ya Israyeli, Hezekiah mwana mwamuna wa Ahaz, mfumu ya Yda anayamba kulamulira. ² Anali na zaka twenti-faivi pamene anayamba kulamulira; analamulira zaka twenti-naini mu Yerusalemu. Amai bake beze Abijah; bezeli mwana mukazi wa Zakaria. ³ Anacitazoyenera pamenso ya Yahwe, anakonkha cisanzo chazamene Davide, anali anacita. ⁴ Anacosa malo yapamwamba, anaononga miyala yaimikila mizati, ana gwesa voimikila Asherah. Anatiola njoka yamene Mose ezeli anapanga, cifukwa banthu ba Israyeli bezeli ku shoka vonukilisa kuli ico; zina yake yeze "Nehushtan." ⁵ Hezekiah anakhulupilira muli Yahwe, Mulungu wa Israyeli, nakuti pambuyo pake kunalibe wingo ezeli ngati eve pamafumu bonse ba Yuda, kapena pa mafumu bezelipo akalibe kukhalapo eve. ⁶ Anagwilira kuli Yahwe, Sanaleke kumukonkha koma anasunga malamulo, yake yamene Yahwe anapasa Mose. ⁷ Ndipo Yahwe anali ndi Hezekiah, konse kwamene anayenda analemela. Anaukira mfumu ya Assyria ndipo sana mutumukile iye. ⁸ Anamenya Afilisti ku Gaza na malile apafupi, kucokela ku nsanja yaolonda malo opotulika yaja. ⁹ Mu caka ca cinai mfumu Hezekiah, cinali caka seveni ca Hosheah mwana mwamuna wa Elah mfumu ya Israyeli, Shalmaneser mfumu ya Assyria analobeleva Samaria ndi kuitenga. ¹⁰ Pa kusila kwa caka ca citatu banatenga, mucaka ca sikisi cah Hezekiah, camene cize caka ca naine ca Hoshea mfumu ya Israyeli; munjila iyi Samaria inatengewa. ¹¹ Pamene apo nfumu ya Assyria anatenga Israyeli nakuyenda ku Assyria naku baika ku Halah, napa mabali pa kamana ku Gozan, na mumalo yaku Medes. ¹² Anacita ivi cifukwa sibanakonkhe mau ya Yahwe Mulungu wao, koma banapwanya cipangano, vosevamene Mose mutumiki wa Yahwe analamula. Banakana kumvela kapena kucita. ¹³ Ndipo mucaka ca fotini cha mfumu Hezekiah, Sennacherib mfumu Assyria anamenya onse malo onse ya malinga anakupoka. ¹⁴ Ndipo Hezekiah mfumu ya Yuda anatuma mau kuli mfumu ya Assyria, wamene ezeli pa Lachish, kuti, "Nakulakwila iwe. Ucoke kuli ine. Ciliconse camene uzaniyuza kucita nizacita." Mfumu ya Assyria inafuna kuti Hezekiah mfumu ya Yuda kuti alipile matalanta yali handiredi ya siliva na matalanta yali feti ya golide. ¹⁵ Na Hezekiah anapasa iye siliva yonse yamene inapezeka mu nyumba ya Yahwe na mosungila za umfumu. ¹⁶ Hezekiah nthawi iyi anakwangwe golide yaku ciseko caku tempeleya Yahwe naku voimila kuja vamene anavika vitali; anapasa golide mfumu ya Assyria. ¹⁷ Koma mfumu ya Assyria anasonkhaniza asilikali ba nkondo ampha, vu kutumanduna na madoda na mukulu wa nkondo waku Lachish kuli mfumu Hezekiah ku Yerusalemu. bana yenda na mendo pansi nakufika ku Yerusalemu. Nakufika pa manzi pa yapamwamba munjira yaku mwaniko amene asoka nyula. ¹⁸ Pamene anaitana mfumu Hezekiah, Eliakim mwana mwamuna wa Hilkiyah, amemne anaona nyumba ya mfumu, na Shebna olemba, na Joash mwana mwamuna wa Asaph, amene anali kulemba mbili. ¹⁹ Anakamba nao kazembe kuti kamba na Hezekiah, yakamba mfumu ikulu ya Assyria, kuti, "Chikhulupiro cako ciloza kuti" ²⁰ Ukamba mau acabebe cabe, kuti kuli umphingu na nkondo, mwaiye ukhulupilira kuti ukile ine. ²¹ Ona ukonda na kukhulupilira ndodo yotyoka iyiya bango. Koma ngati mwamuna asamilako, inkhalila mu manja yake nakubola. Ndiye vamene Farao mfumu ya Egypto ziliku okhulupilira eve. ²² Koma ngati ukamba naine kuti, 'Tikulupira muli Yehwe Mulungu wantu,' simwamene ali pamwamba pa malo na maguwa yamene yanapangiwa na Hezekiah yatengewe, ndipo akamba kwa Yuda na Yerusalemu, 'Mufunika ku pembeza guwa iyi mu Yerusalemu?' ²³ Manje mvelani, nifuna kupasani zabwino kucokera ku mfumu ya Assyria. Mkulu wanga nizakupasa akavalo zikwi ziwili, ngati mwapeza amene afunika kuziyendesa. ²⁴ Mungakane bwanji mkulu wa nkondo monzi wa mone inezi wa mfumu yanga? Mwaika chikhulupilop canu mwa Egypto na nkondo zao na akavalo a nkondo bao. ²⁵ Sininayendepo ine ku mwamba kwa nkondo kulibe Yehwe naku iononga? Yehwe anakamba naine, 'menya malo aya yaononge.' ²⁶ Pamene apo Eliakim mwana mwamuna wa Hilkiyah, na Shebna, na Joah anakamba kuli mukulu wa nkondo, "Nipepha kamba kwa banchito mucitundu ca Aramaic, pakuti tivela. Osakamba naise muchi Yuda pa menso pa banthu amene bali ku malinga." ²⁷ Koma mkulu wa nkondo anati, "Kodi mkulu wanga wa nchito sana kutumire kuli mkulu wa nchito wanga kuti mukambe mau aba? Kodi sana itume kuti bamuna bamene ba nkhalu ku cipupa amene afunika kudya zonyansa zao nakumwa mitundo yao pamodzi naimwe?" ²⁸ Anamulira kazembeyu nakukamba mokuwa mu ci Yuda anati, "Mvelani ku mau ya mfumu ya mfumu ikulu, mfumu ya Assyria. ²⁹ Mfumu inati, 'Musalole Hezekiah akunameni imwe, cifukwa sazakamba ku kupulumusani imwe ku mphamvu yanga. ³⁰ Musalole Hezekiah kuti akupangeni imwe kuti mukulupilire Yahwe, ati "Yahwe azatipulumusa ife zoona, ndipo malo aya sizapasiwa kwa mfumu ya assyria." ³¹ Musamvele Hezekiah, cifukwa izi ndiye zamene mfumu ya Assyria yakamba: 'Mupange mtendele na ine mucoke kuli ine. Aliyense azamwa vakumwa vake vopangiwa kucoka ku mtengo wa mpesha, na manzi yonse ku mkuyu wake na manzi yaku msinje. ³² Uzacita ivi mpka ine nibwele mutengani mupelekani ku malo yaku kwanu, malo yazomela na vinyo wa nyowani, malo ya mkate na mpesha, malo ya azitona na uci, kuti mkhale na moyo osafa.' Musamvele Hezekiah pamene afuna ku kukhani imwe, akuti

'Yahwe azakupulumusani imwe.'³³ Kodi milungu inango ya banthu yaba pulumusa mu manja ya Assyria?³⁴ Ilikuti milungu ya Hamath na Arpad? Ilikuti milungu ya Sepharvaim, Hena, na Ivvah? Kodi banapulumusa Samaria mumanja yanga?³⁵ Pali milungu yonse ya pamalo yano, kodi alipo mulungu anapulumusa chalo cake mumanja yanga? Yahwe angapulumuse bwanji Yerusalemu kucosa mu mphamvu yanga?"³⁶ Koma banthu banali zii sibanayankhe, pakuti mfumu inalamulira , " Osamuyankha iye." ³⁷ Ndipo Eliakim mwana mwamuna wa Hilkiah, amene asebenza mu nyumba ya mfumu; Shebna wolembe; na Loah mwana mwamuna wa Asaph, analembe, anabwela kwa Hezekiah na zobvala zong'ambika, ndipo anamuza eve mau amene wa mukulu wa nkondi anakamba.

Chapter 19

¹ Zinali pamene mfumu Hezekiah anamvela ripoti, anang'amba zobela zake, anabvala masaka, nayenda ku nyumba ya Yahwe. ² Anatuma Eliakim, amene anali mu nyumba yake, na Shebna wolemba, na akulu-akulu anseme, bonse banazivalika masaka, Isaya mwana mwamuna wa Amoz, muneneli. ³ Banakamba kuli eve, " Hezekiah kuti, ' Siku iyi ni siku ya masauso, cizuzulo, na masuso, pakuti bana bafika pa nthawi yo badwa, koma kuli mhamvu kuti ba badwe. ⁴ Cilingati kuti Yahwe Mulungu wanu azamvela mau onse ya mkulu wa nkondo, wamene mfumu ya Assyria mkulu wa nchito wake amutuma atonze Mulungu wamoyo, naku zula mau amene Yahwe Mulungu wanu amvela. Manje ngamulani mapemphero yanu kwa baja bamene bana sala. ⁵ Ndipo ba mfumu Hezekiah bana bwela kuli Isaya, ⁶ na Isaya anabauza beve, " Kambani kuli mukulu wanu; ' Yahwe akamba, " Musayope pali mau mwamvela, yamene uyu wanchito wa Assyria anitukwanilapo ine. ⁷ Onani, nizaika pali eve mzimu, ndipo azamvela mau yena nakubwelela ku malo yakwao. Nizamupanga kuti angwe na lupanga ya mumalo ya kwa." ⁸ Ndipo mkulu wa nkondo anabwela nakupeza kuti mfumu ya Assyria amenyana na Libnah, cifukwa anamvela kuti mfumu ayenda ku Lachish. ⁹ Ndipo Sennacherib anabwela kuti mfumu Tirhakah waku Cush na Egypto anaika pamodzi banthu ku amenyane naye, eve anatuma mthanga kwa Hezekiah. ¹⁰ "Kamba kuli Hezekiah mfumu ya Yuda, 'Musalole mulungu wanu wamene mukhulupirilamo kuminamizzani imwe, kukamba, " Yerusalemu sazapasiwa mmanja ya mfumu ya Assyria." ¹¹ Onani, mwamvela vamene mfumu ya Assyria anacita kuli malo yonse anayaong'onga kosilizilatu. Ndipo muzapulumuswa? ¹² Kapena milungu ya ziko yabapulumusa beve, ziko yamene makolo yanga atate anaononga: Gozani, Haran, Rezech, na banthu baku Eden mu Tel Assar? ¹³ Mfumu yaku Hamah, ilikuti mfumu yaku Arpad, mfumu yaku malo yaku Sepharvaim, Hena, na Ivvah?" ¹⁴ Hezekiah analandila kalata iyi kucokela kwa mesenja ndipo anaibelenga. Ndipo anayenda pamwamba pa nyumba ya Yahwe na kuika kalata pamenso ya Mulungu. ¹⁵ Hezekiah anapempera kuli Yahwe na kuti, " Yahwe wamene akhla pakati, Mulungu wa Israyeli, imwe amene mukhala pakati pa kerabi, imwe mweka Mulungu wa ufumu wa kumwamba na pansi. Munapanga kumwamba na pansi pa calo. ¹⁶ Mvelani matu yanu, na kumvela. Segulani menso yanu, Yahwe, na kuona, naku mvela mau ya Sennacherib, yamene atuma kunyoza Mulungu wa moyo. ¹⁷ Zooni, Yahwe, mafumu ya Assyria yaononga calo cao na malo yao. ¹⁸ Baika milungu yao pa mulilo, pakuti siinalin milungu koma nchito ya banthu amuna na manja yao, mitengo na mwala. Ndipo Assyria baononga zonse. ¹⁹ Koma manje, Yahwe Mulungu wanthu, tipulumuseni ise, nikupemphani, ku mphamvu zake, kuti mafumu yanango yazibe kuti ndimwe, Yahwe, Mulungu mweka. ²⁰ Isaya mwana mwamuna wa Amoz anatuma uthenga kuli Hezekiah, kuti, " Yahwe, Mulungu wa Israyeli akuti, 'Cifukwa wa pemphera kuli ine kukamba za Sennacherib mfumu ya Assyria, nakumvela iwe. ²¹ Aya ni mau yamene Yahwe akamba pali eve: " Namwali mwana mukazi wa Ziyoni nkakhale kuti unyoza naku seka. Mwana mukazi waku Yerusalemu ana pukusa muli wako kuli iwe. ²² Nindani amene waononga naku tukwana? Kuli uyo amene mwakweza na mau yako nakunyamula menso yanu mozikweza? Nakunyoza Oyera yaku Israyeli ²³ Mwa amesinja banu mwacimwila Mulungu, ndipo mkuti, ' Naza mkhondo zanthu nayenda kumwamba pamaphiri, pamwamba pa Lebanon. Nizagwesa utali wa mikungaza na mitengo yosankhiwa ya mlombwa. Niloba futi mngika mukati, mweni mweni mkkati mwa sanga. ²⁴ Nakumba motapa manzi namwa manzi yakunja. Na yumika tumana twa mu Egypto mwa miyendo yanga. ²⁵ Simunamvele kuti ninacitta kudala masiku yaja yakudala? Na sebenza mwa ma masiku ya makolo yanthu sopano nifuna vicitike. Mulipo kuti kucosako ma minzi aya mumalinga ya munja. ²⁶ Onkhalamo: ba mhamvu zing'ono avaliwa naku mvesewa nsoni. Ni voshanga va mu munda vili gilini mauzu a mtenje kapena ma munda, yashokewa yaka libe kukula. ²⁷ Niziba kunkhala pansi kwako, kuyenda kunja kwako, kubwela kwako, naku nizazila kwako kwa nga. ²⁸ Cifukwa ca kunizazukiola kwako kuliine. Cifukwa n thota zaka zamveka kuli ine nizaka mbeza mu mphuno mwako, na cokumwa canga mu kamwa mwako; nizakuikaka kumbuyo, monga unabwelela." ²⁹ Ichi chizankhala cindikilo cako: Cino caka uzadya za molulumukwa, mu caka cibwela mufunika kushanga. Koma mu caka cacitatu mufunika ku shanga nakokolola, mu shange mphesha na kudya zbala zake. ³⁰ Bosala ba Yuda bazaika mizu naku bala zipaso. ³¹ Kucoka ku Yerusalemu osala azacoka, kucokela ku malupili ya Zayoni opulumuka bazabwela. Cofuna ca Yahwe onkhala pakati azacita izi. ³² Pamene apo Yahwe anakamba izi pa mfumu ya Assyria: " Sazabwela mu malo kapena kulusa mkondo pali ponse pazankhala palibe nkhide. Covala pa cifuba, kapena kumanga malo yobisalamo pomenya nkondo. ³³ Njila yamene azabwelelamo niyamene azayendelamo; sazaloba mumalo - alamula Yahwe." ³⁴ Nizabachingiliza malo yano nakuyapulumsa, cifukwa cacifunilo canga na cifukwa ca Davidi mutumiki wanga." ³⁵ Cinabwela pa usiku uja kuti mungelo wa Yahwe anayenda kunja nakumenya malo ya Assyria, kupaya ba nkondo 185,000. Pamene bamuna banauka kuseni-seni, ma thupi yakufa yanali paliponse. ³⁶ Ndipo Sennacherib mfumu ya Assyria anachoka ku Israyeli nakuyenda ku nyumba ndipo anakhala ku Nineveh. ³⁷ Patapita nthawi, pamene anali ku pemphla mu nyumba ya Nisrok

mulungu wake, bana bake bamuna Adrammelek na Sharezer bana mupaya na lupanga. Ndipo banatabila ku malo aku Ararat. Na Esarhaddon mwana wake mwamuna anakhala mfumu.

Chapter 20

¹ Mu masiku aja, Hezekiah anali wodwala pafupi kufa. Ndipo Isaya mwana mwamuna wa Amoz, muneneli anabwela kuli eve, na kukamba kuli eve, " Yahwe akuti, 'ika nyumba yako bwino; cifukwa uzafa, na siuzankhala na moyo.'" ² Ndipo Hezekiah anaika nkhope yake pansi kuciumba naku pemphera kuli Yahwe, kuti, ³ " Napapata, Yahwe, kumbukilani mwamene ninayendela pa menso panu na mtima wanga onse, na vamene ninachita pamenso panu vabwino." Ndipo Hezekiah analira manigi. ⁴ Ndipo Isaya anayenda pakati pa munzi, mau a Yahwe yanabwela kuli eve, kukamba, " ⁵ Bwerera kumbuyo, kakambe kuli Hezekiah, musogoleri wa banth banga, ' Izi ndiye vamene Yahwe Mulungu wa Davidi makolo yako, akamba:" Namvela pemphero yako, ndipo naona kulira kwako. Nili nakukupolesa iwe pa siku ya citatu, ndipo uzayenda pamwamba pa nyumba ya Yahwe. ⁶ Nizaikapo zaka fititini pa umoyo wako, na kupulumusa iwe na malo yano ku manja ya mfumu ya Assyria, na kucingiliza malo yano cifukwa ca kufuna kwanga na Davidi mtumiki wanga.'" ⁷ Ndipo Isaya anakamba, " Tenga laiti ya mtengo wa nkhuu." Anacita ici naika pa pafundo, ndipo anapola. ⁸ Hezekiah anakamba kulin Isaya, " Kodi niciani cizaonesa kuti Yahwe azanipoleso, na kuti niyende ku nyumba ya Yahwe pa siku yacitatu?" ⁹ Isaya anayakha, " Ici cizankhala coonesa kuli iwe kucokela kuli Yahwe, kuti Yahwe azacita monga mwamene akambila. Kodi civilivli cizayenda pasogolo kali teni kapena kumbuyo kali teni? ¹⁰ Hezekiah anayankha, " Nicapafupi kuti civilivli kuyenda pasogolo kali teni. Iyayi, lekani civilivli ciyende kumbuyo kali teni." ¹¹ Ndipo Isaya muneneli analira kuli Yahwe, na kubwelesa civilivli kumbuyo kali teni, kucoka pamene cinayenda pa kwelero ya Ahaz. ¹² Pa nthawi iya Marduk-Baladan mwana mwamuna wa Baladan mfumu ya Babylon anatauma ma kalata na mhaso kuli Hezekiah, cifukwa anamvela kuti anali kudwala. ¹³ Hezekiah anamvela kuli makalata yaja, nakuionesa kuli amesinja bake bonse amunyumba ya mfumu na zinthu zake zonse, sliva, golide, zonukhila na mafuta abwino, nakosungila za nkondo, na vonse vamene vezeli mosungila vinthu. Kunalibe vamene vinali nyumba yake, kapena mumalo ya ulamulilo yake, vamene Hezekiah sanabalangize. ¹⁴ Ndipo Isaya muneneli anabwela kuli mfumu Hezekiah na kumufusa, " Kodi amuna aba bakamban cani? Bacokekela kuti?" Hezekiah anakamba, " Bacoka ku calo cakutali Babylon." ¹⁵ Isaya anafunsa, " Baona ciani mu nyumba mwako?" Hezekiah anayanka, " Baona vonse mu nyumba mwanga. Kulibe vamene sibanaone pavonse vanga." ¹⁶ Ndipo Isaya anakamba kuli Hezekiah, " Mvela ku mau ya Yahwe: ¹⁷ ' Ona, masiku yabwela pamene vonse mu nyumba yako ya ufumu, vamene makolo yako yana bisa kufikila lelo siku yalelo, vizatengewan ku Babylon. Palibe vizasala akamba Yahwe. ¹⁸ Benango bana bako bazatengewa bamene unabala azankhala adindo mu nyumba ya Mfumu yaku Babylon.'" ¹⁹ Hezekiah anakamba kuli Isaya, " Mau a Yahwe yamene akamba niyabwino." Cifukwa anaganiza, " kuti kuzankhala kulibe mtendele na citetezo mu masiku yanga?" ²⁰ Kukamba pa nkani zin zake za Hezekiah, na mhamvu yake yonse, mwamene anapangila mosambila na motandalira, na mwanene analetela manzi mu malo yaja-kodi sivinalembewe mu buku ya mfumu ya zocitika ya Yuda? ²¹ Hezekiah anagona na makolo yake akudala na Manasseh mwana wake mwamuna anakhala mfumu malo mwake.

Chapter 21

¹ Manasseh eze nazaka twavu pamene anayamba kulamulira; analamulira zaka fifite-faivi mu Yerusalemu. Amai bake zina yabo yeze Hephzibab. ² Anacita coipa pamenso ya Yahwe, monga vija vamene anacosa muziko ya Israyeli. ³ Anamanganso malo yapamwamba yamene Hezekiah atate bake banali baononga, nakumanga guwa ya Baal, anapanga Asherah poo, monga Ahab mfumu ya Israyeli ina chitila, anagwada pansi ku nyenyenzi kumwamba nakuzipembeza. ⁴ Manasseh anamanga maguwa mu nyumba ya Yahwe, ngakhale kuti Yahwe ndiye analmulira, " Ni mu Yerusalemu mwamene zina yanga izamveka muyayaya." ⁵ Anamanga maguwa ya nyenyenzi zonse za kumwamba mumalo yabili ya munyumba ya Yahwe. ⁶ Analengesa bana bake kuti bapite mumuliro, anacita voombeza kuombeza na ang'anga vobwebweta naba mene bafuna kuyenda na mizimu. Anacita vambili ku menso ya Yahwe, kulengesa kuti akalipe. ⁷ Anasema cosema ca Asherah camene anapanga, anaika mu nyumba ya Yahwe. Nimwamene umu mu nyumba ya Yahwe anakamba Davidi na Solomon mwana mwamuna wake; anakamba: "' Nimu nyumba umu na mu Yerusalemu, yamene nasankha pam mitundu ya Israyeli, nizaika zina langa kuti inkhalile. ⁸ Sinifuna kupangisa mendo yaba Israyeli kuti yadabwe mu malo yamene ninapasa makolo yao yakudala, Nipepamene bazankhala bosunga malamulo yamene nabapasa, kupitila muli Mose." ⁹ Koma banthu sibanamvele, na Manasseh anaba sogolela beve kucita coipa kupitiliza ziko yonse yamene Yahwe anaononga pamenso pa bana ba Israyeli. ¹⁰ Chakuti Yehova anakamba kupitila mulibakapolo bake baneneli, kuti, ¹¹ "Chifukwa Manase mfumu ya Yuda achita zonyabasa, na zochimwa kuchila bonse ba amonyitisi banali kumbuyo kwache, atengesa na Yuda kuchimwa namafana yake, ¹² ndipo Yehova, Mulungu wa Isilayeli, akamba kuti: onani, nifuna kuchita zoyipa mu Jerusalem na Yuda kuti alionse azanvela, matu yake yonse yake yabili yaza nyinyirika. ¹³ Niza tambulula Yerusalemu coyeselako kumenya Samaria, camene cina sebezese wa ku nyumba ya Ahab; Nizasuka Yerusalemu, monga munthu asukila mambale, asuka naika mopindimuka kuika pansi. ¹⁴ Nizataya bosala botenga banga nabibapa kuli ba adani. Azankhala bovutisiwa ba adani, ¹⁵ cifukwa cakuti bacita coipa kuli ine banikalipisa na ukali, kucokela pamene makolo yao yanacoka mu Egypto, mpaka lelo." ¹⁶ Ndiponso, Manasseh anataya magari yambili ya banthu balipe cimo, mpaka anazalisa Yerusalemu kucoka kwina kufikila kwina futi kufa. Cinali kuikapo pamacimo monga anapanga Yuda kucimwa, monga bana cita coipa kuli Yahwe. ¹⁷ Kukamba pa vinthu vinango Manasseh, zonse zamene anacita, na cimo anacita sizinalembewe mubuku ya zolembewa ya mfumu ya Yuda? ¹⁸ Manasseh anagona na makolo yake ndipo anaikiwa mu munda yamu nyumba yake, mdimba ya Uzza. Amon mwana wake mwamuna anakhala mfumu mumalo mwake. ¹⁹ Amon anali na zaka twenti-wanu pamene anayamba kulamulira, analamulira Yerusalemu zaka tuu. Amai bake zina yabo yeze Meshullemeth; wamene eze mwana mukazi wa Harz waku Jotbah. ²⁰ Anacita coipa pa menso pa Yahwe, Monga Manasseh atate bake banacitilia. ²¹ Amon anakonkha mwamene batate bake banapita na kupembeza mafano, anagwadila kuli ivi. ²² Anasiya Yahwe, Mulungu waba tate bake, sanayende munjila ya Yahwe. ²³ Mtumiki Amon anacita coipa na ku paya mfumu mu nyumba yake. ²⁴ Koma banthu banapaya bonse batonza mfumu Amon, nakupanga Josiah mwana mwamuna wake mfumu mumalo mwake. ²⁵ Pa nkani zina za Amon nazamene anacita, Kodi sizinalembewe mubuku yolembamo vocitika ya mfumu ya a Yuda. ²⁶ Banthu bana muika mu munda yake mdimba ya Uzza, na Josiah anakhala mfumu mumalo mwake.

Chapter 22

¹ Josiah anali nazaka eiti pamene anayamba kulamulira, analamulira zaka feti-wanu mu Yerusalemu. Zina ya bamai bake yeze Jedidah (mwana mukazi wa Adaiah waku Bozkath). ² Anacita camene cizeli coyenera pamenso pa Yahwe. Atate bake Davidi banayenda, sana chinje kapena kuyenda ku liiti olo ku lefuti. ³ Inafika mu mwaka wa eyitini ya Josiya mfumu. anatuma Shapani mwana wa Azaliya mwana wa Meshullamu, mutembi, munyumba ya Yehova, Kuti, ⁴ "Yenda kuli Hilkiyah mukulu wansembe umu'uze kuti apende ndalama zamene zaletewa kachisi bana tenga kubantu. ⁵ Zipasiwe mumanja ya ogwira nchito bebayangana nyumba ya Yehova, ndipo bapase bogwila nchito bali mu nyumba ya Yehova, kti bapange zowonogeka mu tempele. ⁶ Balekeni bapase ndalama kuli opala mapulanga, naomanga, naogula mapulanga ndipo bajube miala bakone tempele." ⁷ Koma kunalibe kubelenga ndalama zamene anapasiwa, cifukwa anazisunga mokhulupilika. ⁸ Hilkiyah wa nsembe mkulu anakamba kuli Staphan olemba, " Napeza buku ya malamulo mu nyumba ya Yahwe." Ndipo Hilkiyah anapasa buku Staphan, ana ibelenga. ⁹ Staphan anayenda nakutenga buku kupasa mfumu, anapeleka ripoti kuli eve kukamba, " Banchito basebenesa ndalama zamene banapeza mu tempele naku pasa bosenza mu tempele nbamene basunga nyumba ya Yahwe." ¹⁰ Pamenso apo Staphan olemba anakamba kuli mfumu, " Hilkiyah wa nsembe mkulu anipasa buku." Ndipo Staphan anaibelenga. ¹¹ Zinali pamene mfumu anamvela mau ya malamulo, anang'amba vobvala vake. ¹² Mfumu inalamulira Hilkiyah wa nsembe, Ahikam mwana mwamuna wa Staphan, Akbor mwana mwamuna wa Micaiah, Staphan olemba , na Asaiah, wanchito wake, kukamba, ¹³ " Yenda ndipo ufunsekuli Yahwe pamalo paine, na bonse banthu na yonse Yuda, cifukwaca mau yamene napeza mubuku iyi. Ukali wake niuukulu Yahwe wamene wayakila ife cifukwa ca makolo batu sibanamvele vamene buku iyi ikamba kuti bakonke vonse vamene vinalembewa pali ise. ¹⁴ Ndipo Hilkiyah wa nsembe, Ahikam, Akbor, Staphan, na Asaiah banayenda kuli Huldah muneneli, mukazi wa Shallum mwana mwamuna wa Tikvah mwana mwamuna wa Harhas, osunga maika vovala (anankala mu Yerusalemu mu kota yanamba tuu), na kukamba naye. ¹⁵ Anabauza beve, " Ivi ndiye vamene Yahwe, Mulungu wa Israyeli, akamba: ' Muuze mwamuna akutumani kuli ine, ¹⁶ Ivi ndiye vamene Yahwe akamba: ' Ona, Niza bwelesa coipa mumalo yano na vonse vonkhalamo, kulingana na vamene vina lembewa mubuku yamene mfumu ya Yuda yabelenga. ¹⁷ Chifukwa mwanisiya nakushokela vonunkila kuti milungu twenangu , chakuti banilengesa kukwiya namachitidwe yeba chita-Koma lu kwiya kwanga kwayasa pamalo aya, ndipo sikuza zimiwa.'" ¹⁸ Koma kuli mfumu ya Yuda, anamitumani kufunsa Chifunilo cha Yehova, Ivi ndiye ve muzayena kumuwuza: "Yehova, Mulungu wa Isilayeli akamba kuti: konkaniza na mau ye ananvela, ¹⁹ chifukwa mutima wako unali wofewa, ndipo chifukwa unazichepesa kuli Yehova , pamene unanvela venina kamba pali aya malo na bonse bebankala mo, kuti bazakankala bwinja na tembelelelo, ndipo kuli ine, naine niminvelani-uku ndiye kulengesa kwa Yehova. ²⁰ Ona, niakuika pamozi na makolo yako, ndipo uaikiwa mumanda mwako mu mtendere. Menso yako siyazaona zonse zoipa zamene nizaika pali malo yano.'" Ndipo bamuna banapeleka uthenga kuli mfumu.

Chapter 23

¹ Chakuti mfumu anatuma bopeleka utenga bana sonkanisila bakulu ba Yuda na Jerusalema. ² Pamene apo mfumu anayenda ku nyumba ya Yehova, naba muna bonse ba Yuda na bonse be bankala mu Jerusalema na enve, na bakulu bang'ono kufikila kuba kulu. Anabelengela mau ya buku yachipangano inapezeka munyumba ya Yehova. ³ Mfumu inaimilira mu comangiwa citali nakupanga cipangano na Yahwe, ktui aayenda na Yahwe na kusunga malomulo, nakukonkha okamba na zolembewa zake na mtima wanthu wonse na moyo wanthu wonse ku vomelea mau ake acipangano zolembewa mubuku. Banthu bonse kusunga cipangano. ⁴ Mfumu analamulira wansembe Hilkihah, wansembe wake, na oimilila pa colobela kuti abwelese vonse vopangiwa na Baal na Asherah, na nyenyei zonse zakumwamba. Ana shoka zonse panja pa Yerusalemu mu munda mu Kirdron vali ndipo banatenga milota yao ku Bethel. ⁵ Anacosa milungu yonse yopangiwa na ansembe amene mfumu ya Yuda anasankha ku shoka zonunkhila pamwamba pa malo ya Yuda mu malo ya Yerusalemu - baja bana shoka zonunkhila kwa Baal, ku zuba na mwezi, mumwamba na ku nyenyezi zonse. ⁶ Anacosa cifanizo copangiwa mu tempele ya Yahwe, kunja kwa Yerusalemu ku Kidron vali ndipo banachishoka kuja. Anaononga ku igaya kunkhala dothi nakuziika ku manda ya banthu ba pansi. ⁷ Anakonza monkhala muja mwa mahule aja bamene benzeli mu nyumba ya Yahwe, kwamene akazi anapanga nyula zosintha ku cifanizo. ⁸ Josiya anachosa ansembe onse mumuzinda wa Yuda naku yipisa malo yapa mwamba pamene wansembe anali kushokela zofukiza, kuchokla ku Geba kufikila ku Beresheba. Anawonga malo yapa mwamaba pa chipata chinali pongenela chipata cha Yohuwa (kazembe wamu muzinda), kumazere kwa chipata cha muzinda. ⁹ Ngakale wansembe wa malo yapamwamba yoja sebenze bovomelesewa kutumikila pa guea ya Yehova mu Jerusalema, banadya muate unalibe vofufumisa bakati pa abale babo. ¹⁰ Josiah anaononga Topheth, yamene ili mu malo ya Ben Hinnom, kuti pasapeeke wopangisa mwana mwamuna kapena mukazi, kupita pa muliro ngati nsembe ya Molech. ¹¹ Anacosa akavalo yamene mfumu ya Yuda inapeleka ku uba. Banali pa malo yenango pafupi na pongenela pa tempele ya Yahwe, pafupi na Nathan - Melek, mdindo. Josiah anashoka ma kavalo yopelekewa ku zuba na muliro. ¹² Josiya mfumu anawononga ma guwa anali pa mutengo wapa chipinda chapa mwamba cha Ahazi, yamene mfumu ya Yuda anapanga, nama guwa yamene manese enze anapanga mu makoti yabili yamu tempele ya Yehova. Josiya anazipwanya muzi dunsu nakuzitaya mu chigawa cha kidroni. ¹³ Mfumu anawononga malo yapa mwamba kumawa kwa Jerusalema, kumazulo kwa lupili lazipupu zamene Solomoni mfumu wa Isilayeli wa anamangila Ashtoreth mafano yonyansa yobaku Sidoni; ya chemoshi, mfano yonyansa ya Moabu; naya Moleki, mfano yonyansa ya bantu ba Amoni. ¹⁴ Anatwola mapilala ya myala muzi dunsu dunsu naku juba mitengo ya Ashira nakuzuya malo yaja nama fupa ya bantu. ¹⁵ Josiya anasiliza kuwononga ma guwa anali ku Bethel napa malo yapa mwamba yamene Jerobomu mwana wa Nebat wamene analengegesa Isilayeli ku chimwa anamanga. Ana shoka guwa na malo yapa mwamba nakuyimenya paka kulukungu. Anashoka mutengo wa Ashira. ¹⁶ Pamene Josiya anayanganila malo, anawona manda anali kumbali kwa lupili. anatuma bamuna kuti batenge mafupa kuchokela mu manda; ndipo anavishoka pa guwa, ina yipisa. Uku kunali kukonkeleza mau ya Yehova yamene muntuu wa Mulungu anakamba, mwamuna wamene anakamba vintu ivi vikali kuchitika. ¹⁷ Ndipo anakamba, "Coumbiwa cabwanji ichi niona?" Amuna amu muzinda anamuza. "Aya ni manda ya munthu wa Mulungu amene anacokela ku Yuda ndipo anakamba pa vinthu vamene mwacita pa guwa ya Bethel." ¹⁸ Ndipo Josiah anakamba, "Ilekeni yeka. Pasapezeke wotenga mafupa." Muyaleke yeka mafupa ya mneneri amene anacoka ku Samaria. ¹⁹ Pamene apo Josiya anachosa manyumba yonse pa malo yapa mwamba yanali mumizinda ya Samaria, yamene mfumu ya Isilayeli anapanga, analengesa Yehova ku kalipa. Anachita kuli benve vamene zinachitiwa ku Bethelo. ²⁰ Anapaya bansembe bonse bapamalo yapamwamba pa guwa ndipo anasjokela yabantu pali zenve. Anabwelela ku Jerusalema. ²¹ Mfumu inalamulira banthu bonse, kuti, "Mucitere Yaweh Mulungu wanu pasika, munga nicolembewa mu buku ya cipangano." ²² Pasiku yaso sinacitikepo kucoka pa nthawi ya owerua ba Israyeli, kapena mu masiku ya mafumu ya Israyeli kapena Yuda. ²³ Koma mu caka ca eitini ca mfumu Josiah pasaka ya Yahwe ina sangalira mu Yerusalemu. ²⁴ Josiya anapilikisa baja banaliku kamba nabo kufa olo namizimu. Anapilikisa futi naba umfwiti, mafano, nazintu zonse zonyase zenzo oneka mu ziko ya Yuda namu Jerusalema, chakuti basimikizike mau ya lamulalo yanali yolembewa anapeza munyumba ya Yehova. ²⁵ Kumbuyo kwa Josiya, kunalibe mfumu munga enve, anayangana kuli Yehova namutima wake onse, oyo wake onse, na mpavu zake zonse, anakonkeleza malamulo yonse ya Mose. Ndipo panalibe mfumu yina munga Josiya inayima pambuyo pake. ²⁶ Koma, Yehova sanachinje kukalipa kwake koyofya, kwe anakalipila Yuda chifukwa cha vonse Manase anachita kulengesa kuti akalipe. ²⁷ Yehova anakamba kuti, "Niza chosa futi na Yuda pamenso panga, mwenachosela Isilayeli, ndipo nizatenga uyu muzinda wenasanka, Jerusalema, na nyumba yamene ninakamba kuti, zina langa lizankalapo." ²⁸ Koma kukamba zankhani zina zokamba pa Josiah, zonse anacita, sizinalembewe

mu buku yazocitika za mfumu ya Yuda? ²⁹ Mu masiku aja, Farao Necho, mfumu ya Egypto, anayenda kumenyana na mfumu ya Assyria ku kamana ka Euphrates. Mfumu Josiah anayenda ku kumana na Necho mu nkondo, na Necho anamupaya pa Megiddo. ³⁰ Wanchito wa Josiah anamutenga pa gareta kucosa pa Magiddo, ku muleta ku Yerusalemu, anamuika mumanda yaje. Ndipo banthu ba mu malo anatenga mwana wake Jehoahaz mwana mwamuna wa Josiah, nakumuzoza eve, kupanga ankhale mfumu mu malo mwa atate bake. ³¹ Jehoahaz anali wa zaka twenti - fili pamene anayamba ku lamumulira, analamulira miyezi fili cabe mu Yerusalemu. Amai bake bake zina yabo yezeli Hamutal; banali mwana mukazi wa Jeremiah waku Lubinah. ³² Jehoahaz anacita coipa ku mnso kwa Yahwe monga makolo bake bonse banacitila. Farao Necho anamuika mu macheni ku Riblah mu malo ya Hamath, Kuti nasalamulile mu Yerusalemu. ³³ Ndipo Necho anamupasa mtenga Yuda makhumi khumi yama talente yasilira talente imozi ya golide. ³⁴ Farao Necho anapanga mwana mwamuna wa Josiah Eliakim mfumu mumalo mwa atate bake Josiah, anachinja zina yake kunkhala Jehoiakim. Koma anatenga Jehoahaz kucoka ku Egypto, na Jehoahaz anafela kuja. ³⁵ Jehoiakim analipila siliva na golide kuli Farao. Ndipo kwanilisa kufuna kwa Farao, Jehoikim kusunghesa malo kubakakamiza pa anthu, mumalo aba kuti apeleke kwaiye siliva na golide monga mwa kufuna kwake. ³⁶ Jehoiakim anali nazaka twenti-faive pamene anayamba kalamulila, analamulila kwa zaka ileveni mu Jerusalema. Zina yaba mai bake inali Zebida; anali mwana wa Pedaia waku Rumah. ³⁷ Jehoiakim anachita zochimwa pa menso ya Yehova, monga zonse makolo bake banachita.

Chapter 24

¹ Mu masiku ya Jehoakim, Nebuchadnezzar mfumu ya babiloni anakukira Yuda; Jehoakim anankala kapolo wake kwa zaka zitatu. Jehoakim anabwelela nakupandukila Nebuchadneza. ² Yehova anatumiza kwa Jehoakim gulu ya akalonga, Asiriya, mowabayiyi na Amonayiti, anatumiza kuli Yuda kuti bawononge. uku kunali kusatira namawu yamene ya Yehova anakamba muli bakapolo bake baneneli. ³ Inali mu mwezi wa Yehova pamene ivi vina bwela kuli Yuda, kuti avichose pamenso oake, chifukwa chama chimo ya masene, nazonse ve anachita, mankope yamu Hebeli yakale yakamba kut, inali chifukwa chakukalipa kwa Yehova, ⁴ ndipo nafuti chifukwa chagazi losalakwa lamene anatila, chifukwa anazuza Jerusalema nagazi losalakwa. Yehova sanali kufunisa kulekelela ivi. ⁵ Kuvintu vina vokumaniza Johoiakim, na vonse ve anachita, sikuti nivolembewa muma buku yamachitidwe ya mfumu za Yuda? ⁶ Jehoiakim anagona namakolo bake, ndipo Jehoiamkim mwana wake anakala mfumu pamalo yake. ⁷ Mfumu ya Iguputo sana kukire nafuti kuchokela mumalo yake, chifukwa mfumu ya babiloni ina gonjesa malo yonse yanali kulamulidwa na mfumu yaku Iguputo, kuchokela ku sinje ya Iguputo kufikila kumumana wa Yufuretisi. ⁸ Jehoiakim anali na zaka eyitini pamene anayamba kulamulila, analamulila mu Jerusalema kwa mwezi itatu. Zina ya bamai bake inali Nehushta; banali mwana wa Elnathan waku Jerusalema. ⁹ Anachita zochimwa pamenso ya Yehova; anachita vamene ba bale bakee banachita. ¹⁰ Pa ntawi ija gulu ya nkondo ya Nebuchadneza mfumu ya Babiloni inakukira Jerusalema nakuzunguluka muzinda. ¹¹ Nebuchadneza mfumu ya Babiloni anabwela mu muzinda pamene basilikali bake bakali kuzunguluka, ¹² ndipo Jehoiaquin mfumu wa Yuda anayenda kuli mfumu ya Babiloni, enve, bamai bake, bakapolo bake, baka kalonga bake, bamalonda bake. Mfumu ya Babiloni anamugwila mu mwaka wake wa eyiti wa lamulila. ¹³ Nebuchadneza anachosa vintu vonse vofunika mu nyumba ya Yehova, na vonse vamu nyumba yachifumu. Anajuba muzidunsa dunsu vintu vonse va golide vamene Solomon mfumu ya Isilayeli anapanga mu tempele ya Yehova, mwamene Yehova anakamba kuti vizachitika. ¹⁴ Anamanga bonse bamu Jerusalema, basogoleli, na bonse ba muna nkondo, ogwilidwa bali teni sauzandi, naba baza bonse naba chisulo. kulibe banasala kupatulila bo saika maningi mu ziko. ¹⁵ Nebuchadneza anamanga Jeroiakim mu Babiloni, kumodzi naba mai ba mfumu, bakazi, bake, bamalonda, na bamuna bakulu ma malo. Anabanga kuchokela ku Jerusalema kufika ku Babiloni. ¹⁶ Bonse bamuna bakondo, seveni sauzandi pamozi, na wani saun=zandi bobaza na bamuna basula, na bonse bayenela nkondo-mfumu wa Babiloni analeta bamua aba nakubangisa mu Babiloni. ¹⁷ Mfumu wa Babiloni anapanga Mattaniah, abale ba batate ba Jehoiakim, mfumu pa malo yake. nakumuchinja zina kunkala Zedekaya. ¹⁸ Zedekaya anali nazaka twenti wani pamene anayamba kulamulila; analamulila kwa zaka ileveni mu Jerusalema. zina ya mai bake banali Hamutal; anali mwana wa Jeremaih waku libnah. ¹⁹ Anachita zochimwa pamenso ya Yehova; Anachita vonse vamene Jehoakim anachita. Kupitila mukukalipa kwa ²⁰ Yehova, ya machitidwe anachitika mu Jerusalema na Yuda, kufikila pamene anabachosa pamaso pake. Ndipo Zedekaya anapandukila mfumu ya Babiloni.

Chapter 25

¹ Pamene apo adani benangu ba Yuda na Benjamini banavela kuti bantu bamene benze mu ukapolo benze kumanga tempele ya yehova, Mulungu wa Isilayeli. ² Bana bwela kuli Zerubabelo naba zikulu bamutundu wamakolo babo. banakamba kuli benve pakuti, monga imwe, timusakila kuli enve kuchokela masiku pamene Esahadoni, mfumu ya Assyri, anatileta pamalo yano." ³ Koma Zebabelo, Jesgua, nabonse bazikulu bamutundu wamakolo wabo, banakamba kuti, "Sindimwe, koma ise timanga nyumba ya Mulungu wat, popeza ndise bamene tiza mangila Yehova, Mulungu wa Isilayeli, monga mwamene mfumu Silalsi waku Perzya analamulila." ⁴ Pamene apo bantu ba malo bana chepesa mpavu mu manja ya bantu baku Yuda; banapangisa kuti bama Judeya bankale na manta ku manga. ⁵ Banalipila balangizi kuti baku muwise volinga vabo. Bana chita ivi vonse pamene pama siku ya Silasi kulamulila kwa mfumu Darius waku Perzya. ⁶ Koma paku yamba kwa kulamulila kwa Ahasueru banalemba vonamizila pamakolo ya Yuda na Jerusalemu. ⁷ Yanali masiku ya Artaxerxesi pamene Bishiamu, Mithredati, tabeli, nabo tandizo babo banalembela kuli mfumu Artaxerxesi waku Pezya. Kalata inalembewa mu Aramiki naku masuliwa. ⁸ Rehumu mukulu wankondo na Shishai mu lembi bana lemba ivi vaso kuli mfumu Artazerzes palo Jerusalemu. ⁹ Kuchoka apo Rahamu mukulu wankondo, Shimishai mulembi, nabengu botandizila, bamene benzeli boweluza nabena akulu akulu amuboma, ma Pezya, bazimuna bochoka ku Erki bochoka ku Susa (ndiye, ma Elamiti)-Bana lemba kalata- ¹⁰ ndipo banagwilizana pamozi nabantu bamene Ashurbanipo wamukulu nawo lemeke anaika mukapolo naku bapatikiza kunkala mu Samaria, pamozi nabonse bamene benze kudela kupitilila musinje. ¹¹ Iyi ndiye fanizilo ya kalata yamene bana tumiza kuli enve: "Kuli mfumu Artaxexesi, wanchito wanu, Azimuna bamu dela kupitilila misinje, lembani ivi: ¹² Mfumu izibe kuti ma Jewi bamene bana yenda kuchoka kuli imwe bana bwela pali ife mu Jerusalemu ku manga muzinda wantota. Basiliza vipupa naku konza maziko. ¹³ Manje lekani mfumu izibe kuti ngati uyu muzinda wamangiwa navi pupa vasiliziwa, sibazapasa chiyamikila, misonko, kapena musonko wamu njila uli onse, ichi chaza ononga mosungilamo mwa mfumu. ¹⁴ Zo-ona chifukwa tadya sauti yamu malo yachifumu, sichoyenela ise kuona manyozo yali yonse kuchitika kuli mfumu. Nichifukwa chaichi tatuma izi luzibisa mfumu ¹⁵ kusakila zolembewa mubaku zatate banu naku punzila kuti uyu nimu zinda wantota wamene uza ononga ma mfumu namadela yaletesa mavuto yambili kuma mfumu nama dela. Ndiye pakati pali bantota kuchoka nakudala ndiye chifukwa chake chamene bana wonongela muzinda. ¹⁶ Tizibisa mfumu kuti ngati muzinda navi pupa vamangiwa, chokonkapo kuzankala kulibe chosalapo chanu mu dela naku pitilila Musinje." ¹⁷ Pamene apo mfumu inabwezela kalata kul Rehumu mukulu wabankondo na Shimishi mulembi nabo tandizila mu Samaria na bonse bamene benzeli mudela naku pilila musinje kuti: "Mutendela unkale wanu. ¹⁸ Kalata yamene mwatuma kuli ine yama suliswa naku belengewa kuli ine. ¹⁹ Lamulo inaikika naine, ndiye banasakila nakupeza kuti pantawi itali muzinda uja unanyamukila pama mfumu, ndipo ntota na kuwukila kunapingiwa muli vamene. ²⁰ Ma mfumu yampavu yana lamulla pali Jerusalemu ndipo banali nampavu pali vonse mu dela nakupitilila musinje. Chiyamiko, musonko wapa njila unalipiliwa kuli benve. ²¹ Manje, pangani lamulo (lamulilani kuti aba bazimuna basiye nakuleka kumanga muzinda uyu paka nipange lamulo. ²² Nankanlani bochenjela kuti musa nyozele izi, nichani kuvomuleza uku Rukule naku leta kuluza chisangako chachifumu? ²³ Pamene lamulo ya mfumu Artaxexesi inabelengewa pali Rehumu, Shimishi mulembi, nabo tandizila babo, bana yenda mwa musanga kunja ku Jerusalemu naku patikiza bama Jewi kuti ba baleke kumanga. ²⁴ Pamene apo nchito ya nyumba ya Mulungu mu Jerusalemu ina imilila paka pali kulamulila kwa mfumu Darius waku Pezya.

Chapter 5

¹ Kuchoka apo Hagsi muneneli na Zakariya muneneli, mubadwo wa Ido, bana nenela muzna ya Mulungu wa isilayeli kulima Jew mu Yuda na Yelusalemu. ² Zerubabelo mwana mwanuna wa Shealtieli na Jeshia mwana mwamuna wa Jozadaki bana nyamuka naku yamba kumanga nyumba ya Mulungu mu Yelusalemu naba zineneli bamene bana batandizila. ³ Chokonkapo Tatenani mukulu wakudela yaku pitili ku kusunje, Shetar-Bozena, nabo mutandizila bana bwela nakumba kuli benve kuti, "Nindani akupasani ulamulilo wakuti mumange nyumba iyi naku siliza vipupa ivi?" ⁴ Nabo banakamba kuti, "Nibandani mazina abo bazimuna bamene bamanga chimangiwa ichi?" ⁵ Koma Inso ya Mulungu inali pali bazikulu babma Jewisshi ndipo adani babo Sibana balekese. Benz kulindila kalata kuti itumiwe kuli Dariusi nakuti lamulo ibwezewe kuli benve pali zokuza izi. ⁶ Iyi ndiye fanizilo ya kalata ya Tatenai Mukulu wakudela yopitila mumana, na Shetar-Bozenai nabo mutandizila mudela yapitilila mumna, yamene bantuma kuli Dariusi mfumu. ⁷ Banatuma kalata, kulembela ivi kuli mfumu Daruisi, "Mutendelel onse unale wako. ⁸ Mfumu izibe kuti tinayenda kudela yaku Yuda kunyumba ya Mulungu wankulu. Imangiwa na myala zikulu nama planga yoikiwa mu vipupa. Iyi nchito ichitika bwini bwino nakukula ikuyenda pasogolo mu manja mwao. ⁹ Tinafunsa azikulu kuti, "Nindani akulamulilani kuti mumange nyumba iyi navi pupa ivi?" ¹⁰ Tinafunsa futi namazina yabo kuti bankle bozibika kuli imwe; mazina yaba zimuna bamene banal bazisogoleli niyolembewa pansi. ¹¹ Umu ndiye mwamene bana tiyankila; bana kuti, 'ndise banchito ba uyo wamene ni Mulungu waku mwamba na ziko yapansi, ndipo tiiman inali yomangiwa zaka zambili zapita pamene mfumu yaikulu ya Isilayelu inaimanga nakuisiliza. ¹² Koma, pamene makolo yatu yana kalipisa Mulungu waku mwamba, ana bapasa mumanja mwa Nebukadineza mfumu yaku Babiloni, mu Kaudiyani, wamene anaononga nyumba iyi nakupeleka bantu mu.....ku babiloni. ¹³ Kunja kwa ichi, mu chaka choyamba pamene Silasi anapasa lamulo kutu nyumba ya Mulungu imangiwemo futi. ¹⁴ Mfumu Silasi inabweza futi vintu va golide na siliva vamene venze vamunyumba ya Mulungu vamen Nebukadineza anabwela achosa kuchokela mu tempele yaku Yelusalemu kupelaka ku Tempele mu Babiloni. Ananibweza kuli wanangu oitaniwa Ssheshibazara, wamene anabwela aika kunkala kazembe. ¹⁵ Anakamba kuli enve kuti, "Tenga vipangizo ivo sebenzesa ivi. Yenda ukavifaja mu tempekle ku Yelusalemu, Nyumba ya Mulungu imangiwemo futi kuja." ¹⁶ Chokonkapo uyu Shebaza anabwela naku ika maziko ya nyumba ya Mulungu mu Yeslusalemu; Apa imangiwa, koma ikalibe kusila. ¹⁷ Manje ngati chinga kondwelese mfumu, chifufuziwe mu nyumba yosungilamo vakudya ku babiloni ngati lamulo kuchokela kuli mfumu Silasi inapasiwa kumanga nyumba iya ya Mulungu mu Yelusalemu. Chokonkapo mfumu Itumiza maganiza yake kuli ise.

Chapter 6

¹ Pamene mfumu Darius analamulira kuti bafufuze za munyumba yosungilamo zithu zakele mu Babylon. ² Mumalo yolimba ya Ecbatana mu Media mpukuto ina pezeka: ³ "Mu chaka choyamba cha mfumu Cyrus, Cyrus anapasa lamulo pa nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu: ' Lekani nyumba imagiwenso ngati malo yapelekelapo sembe, lekani maziko yayikiwe, kotalimpa kwa mikono kunkale sikisi, ⁴ na mizela zitatu za miyala zikulu na mizela za mapulanga yasopano, ndipo mutengo uzalipililiwa na nyumba ya mfumu. ⁵ Sopano bwelesani futi golide na siliva na zinthu za munyumba ya Mulungu, zamene Nebuchadnezzar anabwelesa kuchokela ku tempele mu Yerusalemu na kuzitumiza futi ku ku Yerusalemu. Muli kuziika mu nyumba ya Mulungu.' ⁶ Manje Tatteni, mukulu wa malo ya kupitilila musinje, Shettar-Bozenai, na mabwenzi bamene beze mu malo ya Beyond musinje, bankala patali! ⁷ Siyani nchito ya munyumba ya Mulungu yeka. Mukulu na akuklu Ayuda azamanga nyumba iyi ya Mulungu pa malo pano. ⁸ Ni lamulila kuti imwe muchite ichi kuli akulu Ayuda amene amanga nyumba iyi ya Mulungu: ndalama zochoka kuli zapelekewa kuli mfumu zisebezesewe kuli pila amauna kuti basaleke nchito yabo. ⁹ Vonse vamene vifunika - ngombe zing'ono, mbelele, kapena malaiti zo shokela sembe ya Mulungu wakumwamba, tirigu, soti, vinyu, kapena mafuta kulingana nachilamulo cha ba sembe mu Yerusalemu - bapaseni vonse ivi masiku yonse onsakangiwa. ¹⁰ Muchite ichi kuti bangapeleke sembe kuli Mulungu wakumwamba nakupempelela ine, na bana banga bamuna. ¹¹ Nilamula kuti ngati aliyese apwanya lamulo yamene iyi, mtanda ufunika kuchosewa munyumba mwake na kumupachikapo. Nyumba yake ifunika kupangiwa motayila doti chifukwa chaicho. ¹² Lekani Mulungu wamene alengesa zina yake kukhala yongwesa mfumu iliyonse kapena banthu bamene bakwezeke manja kuchinja lamulo iyi, kapena kuononga nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu. Ine. Darius, ndine nalamula izi. Lekani chichitiwe na khama!" ¹³ Sopano chifukwa cha lamulo yatumiziwa na mfumu Darius, Tattenai, mukulu wamalo, na Shethar - Bozenai na otandiza bake, banachita vonse vamene mfumu Darius analamulila. ¹⁴ Ndipo akulu ba Ayuda banamanga nakukula mu maphunzilo yopelekewa na Hagai muneneli na Zachariah, obadwa mumbuyo mwa Iddo. Bana siliza kumanga molingana ndi lamulo ya Mulungu wa Israyeli na lamulo ya Cyrus, Darius, na Artaxerxes mfumu yaku Persia. ¹⁵ Nyumba inasiliziwa kumangiwa pa siku ya chitatu mumwezi wa Adar, mu chaka cha sikisi cha ulamulilo wa Darius. ¹⁶ Banthu ba Israyeli, ba sembe, alevi, nabonse bagwidwa banakodwela nakupeleka nyumba ya Mulungu osangalala. ¹⁷ Bana peleka ng'ombe tubana tuli handiledi, na handiledi tubana twa mbelele, na ma laiti yali fo handiledi paku peleka nyumba ya Mulungu. Mbuzi twavu zimuna zina pelekewa ngati sembe zauchimo wa Israyeli, imozi pa mutundu ulionse wa Israyeli. ¹⁸ Ba uza ba sembe na Alevi kuti basebezele mumalo osiyana - siyana ya nchito ya Mulungu mu Yerusalemu, monga mwamene zinali zolembewa mubuku ya Mose. ¹⁹ Manje baja bamene bezeli kubisama bana kodwela pasaka pa siku ya fotini mumwezi oyamba. ²⁰ Ba sembe na Alevi banazikoza na kupaya vopeleka pa Pasaka mumalo mwa bonse banali bana bisama, nabeve pamozi. ²¹ Bantu Ba Israyeli bamene banadya nyama za Pasaka bezeli baja banabwelela kuchokela mukubisama ndipo bana ziika pabeka kuzichosa kukufipa kwabantu bamumalo ndipo banafuna Yahwe, Mulungu wa Israyeli. ²² Na chisangalalo manakodwela mwambo wa mukata osapya kwamasiku seveni, chifukwa Yahwe ezeli anabwelesa chisangalalo palibeve na kupindamula mutima wa mfumu Assyria kulimbisa manje yanchito ya nyumba, nyumba ya Mulungu wa Israyeli.

Chapter 7

¹ Manje pambuyo pa ivi, mu ulamulilo wa Artaxerxes mfumu ya Persia, Ezra anabwela kuchokela ku Babylon. Makolo bakale ba Ezra bezeli Seraiah, Azariah, Hilkiah. ² Shallum, Zadok, Ahitub, ³ Amariah. Azariah, meraioth, ⁴ Zerahiah, Uzzi, Bukki, ⁵ Abishua, Phinehas, Eleazar, wameneezeli mwana mwamuna wa Aaron wa sembe mukulu. ⁶ Ezra anabwela kuchokela ku Babylon ndipo eze olemba waluso mumalamulo ya Mose yamene Yahwe, Mulungu wa Israyeli, ezeli apasa. Mfumu inamupasa vivonse vamene ezekufuna chifukwa kwanja ya Yahwe yezze naye. ⁷ Benangu bo badwa mumbuyo ba Israyeli na ba sembe, Alevi, boyimba muma tempele, bo sunga viseko, na bonse banapasiwa nchito yosebena mu tempele bana yenda ku Yerusalemu mu chakka cha seveni cha ulamulilo wa mfumu Artaxerxes. ⁸ Anafika mu Yerusalemu mu mwenzi wa faivi muchaka chamene icho. ⁹ Anachoka mu Babylon pa siku yoyamba mu mwezi oyamba. Paze pa siku yoyamba mu mwezi wa faivi pamene anafika mu Yerusalemu, pakuti kwanja ya Mulungu yeze nayeve. ¹⁰ Ezra anaika mutima wa wake mukubelenga, anatenga, na ku phunzisa malamulo ya Yahwe. ¹¹ Iyi niyamene yeze lamulo yamene Mfumu Artaxerxes anapasa Ezra wa sembe komanso olemba malamulo ya Yahwe wa Israyeli. ¹² "Mfumu yama mfumu Artaxerxes, wa sembe Ezra, olemba malamulo ya Mulungu waku mwamba; ¹³ Ni lamulila kuti aliyense waku Israyeli mu ufumu wanga pamozi naba sembe na Alevi bamene bafuna kuyenda ku Yerusalemu, banga yende. ¹⁴ Ine, mfumu, nabonitandiza banga bali seveni, nikutumani imwe bonse kuyenda kufiunsa za Yuda na Yerusalemukulinga na malamulo ya Mulungu, yamene ili munja mwanu. ¹⁵ Mufunika kubwelesa siliva na golide yamene bapasa mahala kuli Mulungu wa Israyeli, wamene kukhala kwake kuli mu Yerusalemu. ¹⁶ Mupase mahala siliva na golide yonse yamene Babylon yamipasani pamozi na banthu naba sembe ba nyumba ya Mulungu wamu Yerusalemu. ¹⁷ Mungule ng'ombe yonse na mbelele na tirigu na zokumwa zopereka. Muzipeleke pa guwa yamene ili mu nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu. ¹⁸ Yonse siliva na golide mulimonse mwamene yionekela bwino kuli imwe naba longo banu, ku kudwelesa Mulungu wanu. ¹⁹ Muika vintu vonse vinapasiwa mahala kuli eve pa nvhito ya nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu. ²⁰ Chilichose chamene mufuna pa nyumba ya Mulungu, mulolewa kusebezesa ndalama zanga. ²¹ Ine, mfumu Artaxerxes, napasa lamulo kuli bonse bosunga ndalama mumalo monse yakumazulo kwa msinje wa Euphrates, ku pasa vili vonse vamene Ezra afuna kuli imwe vonse, ²² ma siliva yama talent 100, matumba 100 ya tirigu, nama botolo 100 ya vinyu, na muchele wambili. ²³ Chili chonse chilamulo chochokela kuli Mulungu wa kumwamba, muchichita mozipeleka mu nyumba mwake. Chifukwa nichani ukali wake ubwelele mumalo yanga na bana banga bamuna? ²⁴ Tibazibisa zaimwe kuti musaike msonkho kapena misonkho pali ba sembe, Alevi, oyimba, osunga ziseko, kapena bantu baikiwa kuchita nchito mu tempele na banchito ba munyumba ya Mulungu. ²⁵ Ezra, na nzeru zamene Mulungu akupasa, ufunika kusankha ogamula na boweluza ku gamula banthu bonse baku mazulo kwa msinje wa Euphrates, na kutumikila bonse bamene baziba malamulo ya Mulungu wako. Ufunika ku phunzisa bamene sibaziba malamulo. ²⁶ Aliyense wamene sakonka mofikapo malamulo ya Mulungu kapena ya mfumu afunika kulangiwa, kaya ku payiwa, kumuthamangisa, kupokewa vonse vinthu, kapena kumangiwa. ²⁷ Yamikani Yahwe, Mulungu wamakolo bathu, wamene anaika vonse mumutima wa mfumu kuti nyumba ya Yahwe mu Yerusalemu ilemekezeke, ²⁸ na kuikilako chipangano chachikulupiliko chake kuli mfumu, otandiza na bonse botumikila ba mphanvu. Na limbikisiwa na kwanja ya Yahwe Mulungu wanga, ndipo naitanisa pamozi basogoleri baku Israyeli kuyenda naiine.

Chapter 8

¹ Aba nibasogoleli ba makolo bama banja bamene bana choka mu Babylon naine pa nthawi ya ulamulilo wa mfumu Artaxerxes. ² Pa bobadwa mumboyo ba Phinehas, Gershom. Pa bobadwa mumboyo ba Ithamar, Daniel. Pa bobadwa ba David, Hattush. ³ Pa bobadwa mumbuyo ba Shecaniah, wamene eze kuchokela kubobadwa mumbuyo ba Parosh, Zachariah, nayeve beze 150 mamuna bolembewa mzera wobadwiala. ⁴ Pa bobadwa mumbuyo ba Pahath-Moab, Eliehoenai mwana mwamuna wa Zerahiah na eve beze bamuna 200. ⁵ Pa bobadwa mumbuyo ba Zattu, Ben Jahaziel na eve beze bamuna bali 300. ⁶ Pa bobadwa mumbuyo ba Adin, Ebed mwana mwamuna wa Jonathan na eve beze bamuna 50. ⁷ Pa bobadwa mumbuyo ba Elam, Jeshaiiah mwana mwamuna wa Athaliah na eve beze bamuna 70. ⁸ Pa bobadwa mumbuyo ba Shephatiah, Zebadiah mwana mwamuna wa Micheal na eve beze bamuna 80. ⁹ Pa bobadwa mumbuyo ba Joab, Obadiah mwana mwamuna wa Jehiel na eve beze bamuna 218. ¹⁰ Pa bobadwa mumbuyo ba Bani, Shelomith mwana mwamuna wa Josiphiah na eve beze bamuna 160. ¹¹ Pa bobadwa mumbuyo ba Bebai, Zechariah mwana mwamuna wa Bebai na eve beze bamuna 28. ¹² Pa bobadwa mumbuyo ba Azgad, Johanan mwana mwamuna wa Hakkatan na eve beze bamuna 110. ¹³ Banja ba obadwa mumbuyo ba Adonikam banabwela pambuyo. Aya ndiye yeze mazina yabo: Eliphelet, Jeuel, Shamaiah ndipo nabeve beze nabamuna 60. ¹⁴ Pa bobadwa mumbuyo ba Bigvai, Uthai na Zaccur na beve bezeli nabamuna 70. ¹⁵ Ninaika pamozi bazaulendo pa ngalande yoyenda ku Ahava, ndipo tinankalapo masiku ya tatu. Nina funsa-funsa bantu na ba sembe, koma sinapeze aliwonse obadwa mumbuyo mwa Alevi kuja. ¹⁶ Mwaicho ninaitana Eliezer, Ariel, Shemaiah, Elnathan, Jarib, na Elnathan na Nathan, Zachariah, na Meshullam-bamene beze basogoleli-na Joiarib na Elnathan-bamene beze bophunzisa. ¹⁷ Mokokhapo ninabatuma kuli Iddo, musogoleli mu Kasiphia. Ninabauza vokamba kuli Iddo na banja yake, ba nchito ba mutempele bonkala mu Kasiphia, kuti, batitumile ise banchito ba nyumba ya Mulungu. ¹⁸ Motelo banatitumile ise mukwanja ya Mulungu mwamuna zina yake Sherabiah, mwamuna wazeru. Ezeli obadwa mumbuyo wa Mahli mwana mwamuna wa Levi waku Israyeli. Anabwela na bana bamuna 18 nabale. ¹⁹ Nayeve kunabwela Hashabiah. Kwezeli futi Jeshaiiah, umozi wabo badwa mumbuyo ba Merari, naba bale na bana bamuna bawo, bamuna 20 pamozi. ²⁰ Pa bonse abo banapasiwa kusebezela mutempele, bamene David naba kulu banapasa kusebezela Alevi: 200, aliynense anapasiwa kulingana namazina. ²¹ Manje analengeza kusala kudwa pa cigwa ca Ahava kuzzichepesa pamenso ya Mulungu, kufuna njila yasitileti kuchokela kuli eve, bang'ono batu na vonse vintu vatu. ²² Ninabwela soni ku kupempa bankondo kapena akavaro kuli ba mfumu kuti batichingilileko kuli badani bathu munjila, pakuti tinali takamba kuli ba mfumu, 'Kwanja ya Mulungu wantu ili naise bonse bofuna eve muchilungamo, koma mhamvu na ukakli wake uli nabo bonse bamene bama muibala eve.' ²³ Sopano tinasala kudwa na kumufuna-funa Mulungu pali ivi, na kupempa kuli eve. ²⁴ Mokokhapo ninasanka bamuna 12 kuchokela mu ofesi ya basembe: Sherebiah, Hashabiah, na benangu bali 10 balongo. ²⁵ Nina pima siliva, golide, na vintu na zopelaka za munyumba ya Mulungu yamene mfumu, nama kasela na bachito, nabonse ba Israyeli banali bapeleka mahala. ²⁶ Ndipo nina pima mu manja bwabo ma talenti ya siliva 650, matalenti ya vintu va siliva 100, matelenti ya golide 100, ²⁷ mbale 20 za golide zamene zeze pamozi ze zokwana 1000 na mikuwa yopukutiwa bwino ibili yooneka bwino ngati golide. ²⁸ Ndipo anakamba kulibev, "Nimwe bozipoleka kuli Yahwe, na vintu vonse, na siliva na golide ni sembe yopeleka mukufuna kwanu kuli Yahwe, Mulungu wamakolo banu. ²⁹ Muvilanganile na kuvisunga bwino mpaka mwavipima mukalibe kupeleka kuli ba sembe, Alevi, ndi basogoleli ba mabanja yamakolo banu baku Yerusalemu muvipinda vamu nyumba ya Mulungu." ³⁰ Ba sembe, Alevi banavomela kupima siliva, golide, na vintu mumalo mwake nakuzipeleka ku Yerusalemu, ku nyumba ya Mulungu wantu. ³¹ Tinayenda kunja kwa ngalande ya Ahava pa siku ya tweve mumwenzi woyamba kuyenda ku Yerusalemu. Kwanja ya Mulungu wantu ili paliise; anati chingiliza ise ku kwanja ya bandani bantu na bonse bamene banabisama mu njila. ³² Manje tinangena mu Yerusalemu ndipo tinankala masiku yatau. ³³ Ndipo pa siku ya fo siliva, golide, na vintu vonse vinapimiwa panja pa nyumba ya Mulungu wantu, kungena mumanja mwa Meremoth mwana mwamuna wa Uriah wa sembe. Na eve eze na Eleazar mwana mwamuna Phinehas, Jozabad mwana mwamuna wa Jeshua, na Noadiah mwana mwamuna wa Binnui mu Levi. ³⁴ Namba ya kulema kwavonse inazibika. Vonse vopimiwa vinalembewa pathawi ija. ³⁵ Bamene banabwela kuchoka ku ukapolo, bantu bamene banali batamangisiwa, banapeleka sembe zoshoka kuli Mulungu wa Israyeli: mabulu 12 kuli Israyeli yonse, ma ram yali 96, mbelele zili 77, na mbuzi zimuna zili 12 kunkhala chopeleka chauchimo. Vonse vezeli sembe yoshoka ya Yahwe. ³⁶ Manje banapasa lamulo ya mfumu ku bakulu ba mfumu bonse na ma mkazembe bonse baku mazulo kwa msinje wa Euphrates, ndipo bana tandiza bantu na nyumba ya Mulungu.

Chapter 9

¹ Pamene ivi vintu vinachitiwa, bakulu-kulu banabwela kuli ine na kumba, "Bantu ba mu Israeyli, ba sembe, na ba Levi sibana zichose pakati pabantu ba ku malo yenangu ndipo kuipa kwabo: Canaaites, Hittites, Perizzites, Jebusites, Ammonites, Moabites, Egyptians, Amorites. ² Pakuti batenga benengu pa bana bawo bakazi na bamuna, na kusakaniza bantu boyela na bantu baku malo yenangu, na bakulu-bakulu nabasogoleli bakala balli pasogolo mukusa kuluphilika. ³ Pamene ninabwela ivi, ninang'amba pakati vovala vanga na mkanjo ndipo ninachosa sisi kumuntu wanga na ndemvu, ndipo ninankala pansi, kusokonezeka. ⁴ Bonse bamene bazeli kunjenjemela pa mau ya Mulungu wa Israyeli pakusakulupilika banabwela pamozi kuli ine pamene neze pansi na soni kufika mumazulo. ⁵ Koma pasembe yamumazulo nina nyamuka pamene neze nasoni muvovala vanga vong'ambika na mkanjo, ndipo ninagwada na kuika manja yanga kuli Yahwe mMulungu wanga. ⁶ Ninakamba, "Mulungu wanga, Nili na soni kuyanganisa chiso changa kuli imwe, chifukwa mphulupulu pamuntu patu nizambili, na kulakwa kwathu kufika kumwamba. ⁷ Kuchokela kumasiku yamakolo bantu kufikila lelo tankala mu mulamndu ukulu, mafumuy yantu, naba sembe batu banapasiwa mumanja yamafumu bapachalo chino, kulupanga, kuukapolo na zonfunika ndipo viso vantu vili nasoni, monga tinalili lelo. ⁸ Koma pa nthawi ing'ono, chifundo cha Yahwe Mulungu wantu abwelesa bopulumuka bang'ono na kuti pasa ise phazi mumalo yake yoyela. Ivi vezeli va Mulungu wantu kusekungula menso yantu na kuti pasa ise kupumula pang'ono kuukapolo. ⁹ Pakuti ndise bakapolo, koma Mulungu wantu sana tiibale ise koma akilako chipangano cha kukulupilika kuli ise. Achita ichi mumenso ya mfumu yaku Persia kuti ise ati pase mphanvu yasopano, kuti timange futi nyumba ya Mulungu na kuchosa muchiwonongeko. Anachita ichi kuti atipase nkoma yochingilila mu Judah na Yerusalemu. ¹⁰ Koma manje, Mulungu wantu, tingakambe chani pambuho paichi? Taibala malamulo yanu, ¹¹ malamulo yamene munapasa banchito banu baneneli, pamene munakamba, "Malo yano yamene mwangena kuti mutenge siyoyela. Niyoiipisiwa na bantu bamalo yazoyipa. ¹² Manje osapasa bana banu bakazi kubana bao bamuna; osatenga bana bao bakazi kupasa bana banu bamuna, ndipo osasakila mutendele wao na ubwino wabo, kuti munkale bolimba na kudya vabwino vamu malo, manje muzalenga bana banu kukhala nazo nthawi yonse." ¹³ Koma pambuyo pavonse vinabwela pali ise chifukwa chama voipa vamene tize kuchita na unyengo ukulu wantu - pakuti, Mulungu wantu, atilekelela kusaweluzika kwathu naku tileka kupulumuka - ¹⁴ kodi tipwanye malamulo na kupanga vikwati vosakanizana nabantu aba boipa? Simuzakalipa na kutipaya ise kuti kusasale aliyense, aliyense kutaba? ¹⁵ Yahwe, Mulungu wa Israyeli, ndimwe boyela, pakuti tasala ise bopulumuka bang'ono pa siku ino. Onani! Tili pano pali imwe mu uchimo wantu, kulibe wamene anga imilile pali imwe chifukwa chaichi.

Chapter 10

¹ Pamene Ezra anapempela na kulapa, analila nakuziponya pansi pa nyumba ya Mulungu. Bantu bambili ba Israyeli bamuna, bakazi, na bana banakumana pali eve, pakuti bantu beze kulila maningi. ² Shekariah mwana mwamuna wa Jehiel obadwa mumbuyo mwa Elam anakamba, "Ise tankala osakulupililika kuli Mulungu wantu ndipo takwatila bakazi bakwinangu kuchokela kubantu baku malo yenangu. Koma ngakale izi, kukali chiyembekezo pali Israyeli. ³ Manje lekani tipange chipangano na Mulungu wantu kutuma bakazi bonse na bana bao kuchoka kuno kulingana na mwamene Ambuye bakambila na bamene bakakonka malamulo ya Mulungu wantu bama njenjemela, ndipo tileke chichiteke kulingana na malamulo. ⁴ Nyamukani, pakuti ichi chintu chifunika imwe muchichite, ndipo tili naimwe. Nkalani bolimba na kuchita ichi." ⁵ Ndipo Ezra anauka nakupanga ba sembe, Balevi, na bonse ba Israyeli lonjeza kuchita munjila yamene iyi. ⁶ Manje bonse bana panga lumbilo ya ulemu. Ndipo Ezra ananyamuka kuchokela kusogolo kwa nyumba ya Mulungu na kuyenda ku zipinda za Jehohanan mwana mwamuna wa Eliashib. Sanadye mukate uli wonse kapena kumwa manzi, chifukwa ezeli kulila zokhuza kusakulupililika kwa bamene bezeli mu ukapolo. ⁷ Pamene banatuma mau mu Yuda na Yerusalemu kubantu bonse banachoka kuukapolo kuti bakumane mu Yerusalemu. ⁸ Aliyense wamene sana yende kumasiku yatatu kulingana namalamulo yabakulu-bakulu banataya vintu vonse vabo ndipo bana chosewa kukukumana kwa bambili bantu bazeli babwela kuchokela kuukapolo. ⁹ Manje bamuna bonse ba Yudah na Benjamin banakumana mu Yerusalemu masiku yatatu. Weze mwezi wa naine pasiku ya 20 ya mwezi. Bonse bantu banankala pamalo yakulu pa nyumba ya Mulungu, kunjenjemela chifukwa chaichi na chifukwa cha bvula. ¹⁰ Ezra wa nsembe anakamba. "Imwe mweka mwapanga mulandu. Munankala nabakazi bakwinangu kuikilako uchimo wa Israyeli. ¹¹ Koma manje pasani matamando kuli Yahwe, Mulungu wamakaolo banu bakale. Chokani palibantu bakumalo na bakazi bakwinangu." ¹² Bonse banakumana banayanka kumpunda, "Tizachita mwamene mwakambila. ¹³ Koma, palibantu bambili, nafuti ni nthawi yamvula. Tilibe mphamvu zoimilila panja, ndipo ino siskiu yoyamba kapena yachibili yanchito, pakuti tachimwa manigi pakanakni iyi. ¹⁴ Manje lekani bakulu bayimilile kukumana konse. Lekani bonse bamene balola bakazi bakwinangu kunkala mu siti yantu babwele panthawi yamene izayikiwa naba kulu ba siti nabo weluza kufikila kupya kwa mtima kwa Mulungu wantu kutachoka pali ise." ¹⁵ Jonathan mwana mwamuna Asahel na Jahzeiah mwana mwamuna wa Tikvah banasusa ichi, na Meshullam na Shabbethai ba Levi banavomeleza ichi. ¹⁶ Motero bantu bamene banabwelela kuchaka kuukapolo banachiyta ichi. Ezra wasembe anasanka bamuna, basogoleli muma banja yamakolo yakale na manyumba - bonse nama zina yabo, banaona pankani iyi pasiku yoyamba ya mwezi wa 10. ¹⁷ Kufika pa siku yoyamba ya mwezi bana siliza kupeza bamuna bamene baze bankala nabakazi bakwinangu. ¹⁸ Pakati pabo badwa mumbuyo ba basembe pezeli baja bamene banankala nabakazi bakwinangu. Pakati pabobadwa mumbuyo ba Yeshua mwana mwamuna wa Jozadak na balongo bamuna bake peze Maaseiah, Eloiezer, Jarib, na Gedaliah. ¹⁹ Motelo beze bolimbikila kutuma bakazi bao kunangu. Chifukwa beze bolakwa, banapeleka khosa kuchokela pa gulu yakhosa za pakuti bezeli bolakwa. ²⁰ Pakati pa bobadwa mumnuyo ba Immer: Hanani na Zebadiah. ²¹ Pakati pa bobadwa mumbuyo ba Harim: Maaseiah, Elijah, Shemaiah, Jehiel na Uziah. ²² Pakati pabobadwa mumbuyo ba Pashhur: Elioenai, Maaseiah, Ishmael, BNethanel, Jozabad, na Elasa. ²³ Pakati pa ba Levi: Jozabad, Shimei, Kelaiah - peze, Kelita, Pethahiah, Yudah, na Eliezer. ²⁴ Pakati paboyimba: Eliashib. Pakati pabo londa zipata: Shallum, Telem, na Uri. ²⁵ Pakati pabonse ba Israyeli - pakati pabobadwa mumbuyo ba Parosh: Ramiah, Izziah, Malkijah, Mijamin, Eleazar, Malkijah, na Benaiah. ²⁶ Pakati pabobadwa mumbuyo ba Elam: Mattaniah, Zechariah, Jehiel, Abdi, Jeremoth, na Elijah. ²⁷ Pakati pabobadwa mumbuyo ba Zattu: Elioenai, Eliashib, Mattaniah, Jeremoth, Zabad, na Aziza. ²⁸ Pakati pabobadwa ba Bebai: Jehohanan, Hananiah, Zabbai, na Athlai. ²⁹ Pakati pabobadwa mumbuyo ba Bani: Meshullam, Malluk, Adaiah, Jashub, na Sheal Jeremoth. ³⁰ Pakati pabo badwa mumbuyo ba Pahath - Moab: Adna, Kelal, Benaiah, Maaseiah, Mattaniah, Bzalel, Binnui, na Manasseh. ³¹ Pakati pabobadwa mumbuyo ba Harim: Eliezer, Ishijah, Mulkijah, Shemaiah, Shimeon, ³² Benjamin, Malluk, and Shemariah. ³³ Pakati pa bobadwa mumbuyo ba Hashuna: Mattenai, Mattattah, Zabad, Eliphelet, Jeremai, Manasseh, and Shimei. ³⁴ Pakati pa bobadwa mumbuyo ba Bani: Maadai, Amram, Uel, ³⁵ Benaiah, Badeiah, Keluhi, ³⁶ Vaniah, Meremoth, Eliashib, ³⁷ Mattaniah, Mattenai, na Jaasu. ³⁸ Pakati pabobadwa mumbuyo ba Binnui: Shoimei, ³⁹ Shelemiah, Nathan, Adaiah, ⁴⁰ Maknadebai, Sheshai, Sharai, ⁴¹ Azarel, Shelemiah, Shemariah, ⁴² Shallum, Amariah, Joseph. ⁴³ Pakati pa bobadwa mumbuyo ba Nebo: Jeiel, Mattithiah, Zabad, Zebina, Jeddai, Joel, and Benaiah. ⁴⁴ Bonse aba bezeli banatenga bakazi bakwinangu ndipo banankala nabana nabo.

Nehemiah

Chapter 1

¹ Mau ya Nehemiya mwana Hakaliya: Manje Zinachitika mu mwezi wa chisilevu, mu mwaka wa twenti, pamene ni ali mu linga ya susa, ² pamene umozi wa abale, Hanani, na bamuna benangu ba Yuda bana bwela, ndipo nina bafuna pali Ayuda, banasala potaba, bamene banatba kuchokela ku ukapo, napli Yelusalemu. ³ Bana kamba kuti kuli ine, "Baja balimuchigao bana pulumuka ukapolo bali muma vuto yakulu na manyazi chifukwa koma ya Yelusalema yaseguliwa, na zipata za shokewa na mulilo." ⁴ Pamene ninanvela mau aya, ninankala pansi nakulila kwamasiku ninapitiliza kumva chisoni na kusala kudya na kupempela kuli Mulungu wakumwamba. ⁵ Ninakamba kuti, "Chonde ini kupempani, Yehova, Mulungu wa kumwamba, Mulungu mukulu na vodabwisa, wamene asunga chipangano na chikondi choyimilila kuli bamukonda nakusunga malamulo yake. ⁶ Segulani monse yanu na matu yanu yankale ya cheru kuti munvele ma pampelo manje kuli imwe muzuba na usiku pa bantu ba Isilayeli bakapolo banu. Niwulula machimo ya bantu ba Isilayeli, yamene banachimwila imwe. Tonse ine naba munyumba ya batate tina chimwa. ⁷ Tachita zochimwa kuli imwe, ndipo sitina sunge malamulo, malangizo, na malamulo yamene unalamulila Mose. ⁸ Chonde kumbukilani mau munalamulila kapolo wanu Mose, "ngati muchite zosa kulupilika, niza kuwazani pakati pa bantu, ⁹ Koma ngati mwabwelela kuli ine na kukonka ma lamulo yanga nakuya chita, nangu bantu banu banali bo mwazikana pansi pa tambo yakutali maningi, nizakaba sonkanisa kuchokela kuja nakubaleta ku malo kwamene ninasanka kuti zina langa linkale." ¹⁰ Manje nibakapolo bako ndipo nibantu bako, bamene unapulumusa na mpamvu zako na kwanja kwako kolimba. ¹¹ Chonde, nikupempani, Mulungu, matu yankale yochera ku pampelo bakapolo bamene basangalala kulemekeza zina lanu. Manje pambanisa kapolo wako lelo, naku mulangiza chifundo pamenso ya mwamuna uyu." Ninali kusebenza kupeleka chiko kuli mfumu.

Chapter 2

¹ Mumwezi wa Nisani, mumwaka wa twenti wa Artaxerxes mfumu, anasanka vinyu, ndipo ninatenga vinyu nakupasa mfumu. Manje sininakalepo wachisoni pamenso pake. ² Koma mfumu anakamba kuti kuli Ine, "Nichani pachisoni pamenso pako? suwoneka monga wodwala. Ichi nichisoni chakumutima." Ndipo nannkala na manta maningi. ³ Ninakamba kuti kuli mfumu, "mfumu inkale kwamu yayaya! Sikuzankalila wachisoni bwanji pamenso panga? muzinda, malo ya manda ya batate banga, yagora ma mawonongeka, nazipata za wonegeka na mulilo." ⁴ Ndipo mfumu anakamba kuti kuli ine, "Nichani chamene ufuna kuti nichite?" Ndipo nina pempela kuli Mulungu waku mwamba. ⁵ Ninayanka kuli mfumu, "ngati chiwoneka mushe kuli mfumu, ndipo ngati kapolo wanu achita zamushe pamenso panu, munganitume kuli Yuda, kumuzinda wa manda batate banga, chakuti nika yimange nafuti. ⁶ Mfumu ananiyanka (ndipo mfumu mukazi analikale pambali pake), "Uzankala kutali bwanji ndipo azabwelela liti?" mfumu anakondwela kunituma pamene ninamupasa ntawi yoikika. ⁷ Ndiponso ninakamba kuti kuli mfumu, "ngati nichokondwelesa kuli mfumu, nipsaiwe nkalata yaba kazembe bamu chigawo chopitilia mumana chakuti bakanivomelese kuti nipite muma madera yawo pamene niyenda kuli Yuda. ⁸ Kunkala nafuta na nkalata ya Asafiwosunga kalango yamfumu, chakuti anganipase mataba yopangila ma mataba ya linga pansongolo pa tempele naku koma yamuzinda, nayamunyumba mwanene ninkala." Ndipo chifukwa kwanja kwamushe kwa Mulungu kunali pali ine, mfumu ananipasa zamene nina pempa. ⁹ Nina bwela kuli Kazembe mu chigawo chopitilila mumana nakumupasa nkalata yamfumu. Manje mfumu enze ananitumana olamulila gulu langondo nabokwela pama ichi. ¹⁰ Pamene Sanbalate waku Holomayiti na Tobiya waku Amonayiti kapolo anavela, sibana kondwele maningi kuti winangu anabwela wamene enzo sakila tandizo kubantu ba Isilayeli. ¹¹ Nina bwela ku Yelusalema ndipo ninankala kwa masiku yatatu. ¹² Ninanyamuka usiku, Ine nabamuna bang'ono. Siniwuze ulionse zamene Mulungu enze anafaka mumutima wanga kuti nichitile Yelusalemu. Kunalibe vinyama kuchoselako yamene nenze ninankwela. ¹³ Nina yenda panja usiku kupila kuchipata chachigwa, kupila ku chinsime cha nkandwe naku chipata cha ndowe, nakuyenda koma ya Yelusalemu, yamene inali yowonongeka nakuseguliwa, ndipo zipata zamitingo zina wonogewa namulilo. ¹⁴ Ndipo nina yenda kuchipata cha kasupa naku ziwe ya mfumu. Malo yanalu yang'ono kutizinyama nezeninankwela zipite. ¹⁵ Choncho ninayenda panja usiku kupila ku chigwa nakuyendela koma, ndipo ninabwelela nakungenela kuchipata cha chigwa, ndipo nina bwelela. ¹⁶ Wolamulila sibana zibe kwamene neze nina yenda nangu zamene nina chita, nenze nikalibe kubazibisa ba Yuda, nangu ansembe, nangu olemekezeka, nangu bolamulila, nangu ponse banachita chinto. ¹⁷ Ninakamba kuti kuli benve, "mwayawina mavuti yamene tilimo, mwamene Yelusalemu agona mowonogeka nazipata za wononogeka namulilo. Bwelani, tiyeni tiamnge koma ya Yelusalemu. Ndipo sitizanka nafuta mulichamanyazi." ¹⁸ Nina bauza kuti zanja la mushe la Mulungu wanga inali pali ine ndipo namwau yamene mfumu ananiwiza. babakmba kuti, "Tiyene tinyamuke nakumanaga." Ndipi bana limbisa manja yawo nchtio yamushe. ¹⁹ Koma pamene Sanbalate mu Horomiyiti, na Tobiya Kapolo wa Amonayiti, na Geshemu mu Arabiyoni banavwela, bana nyoza nakutilangiza nyoza, nakukamba kuti, "Muchita chani? Muli kuwikira mfumu?" ²⁰ Ndipo ninabayanka, "Mulungu wakumwamba azatipasa pambanisa. Ndise bakapolo bake ndipo tiza nyamuka naku manga. Koma mulibe gawo, mulbe ufulu, mulibe mbili yakale mu Yelusalemu.

Chapter 3

¹ Ndipo Eliashib mukulu wansembe ananyamuka naba bale bake bansembe, banamanga chipata cha nkhusa. bana ipatula nakufaka chiseko pa malo. Bana ipatula kufikila ku tawa ya handiredi nakufika ku tawa ya Haraneli. ² Kufupi nayenve bamuna bamu Jriko banali kusebenza, kufupi nabenze Zaka mwana mwamuna wa Imri anali kusebenza. ³ Bana ba Hassenah bana manga chipata cha nsomba. barachipangila matabwa. nakufaka chiseko, nama bawuti namipiringizo. ⁴ Meremoti anakoza gawo inakonkapo. Nimwana wa Uriya mwana wa Hakkozi. ⁵ Pafupi nabeneve Meshullamu ana konza. Nimwana wa Berechiah mwana wa Meshezabel. Pafupi kwabenve Zadoki anakonza. Nimwana wa bwana. Pafupi nabenze ba Tekoyiti banakonza, koma olemkeza bawo banakana kuchita nchito yamene banalamilidwa kuli woyanganila awo. ⁶ Joirada mwana wa Paseah na Meshullamu mwana wa Besodeiah anakonza chipata chakudala. Banaipangila matabwa, nakuyika chiseko, nama bawuti namipiringizo. ⁷ Pafupi kunlai bamuna bochokela kuli Gibiyoni na Mizpa-Melatiah mu Gibiyoni na Jodani mu Meronotayiti-mupando wachifumu wa kazembe wamuchigawo chopilila mumana. ⁸ Pafupi naye Uzziel mwana wa Harhaiah, omwe wabosula golide, anakonza, ndipo pafupi nayenze kunali Harhaiah, wopanga mafuta onukila. Bana manga Yelusalemu kufikila ku khoma lotakata. ⁹ Pafupi nabenze Rephaiah mwana Hur anakonza. Anali woyanganila hafu ya disitilikiti mu Yelusalema. ¹⁰ Pafupi nabenze Jedaiah mwana wa Harumaph anakonza kufupi nanyumba yake. Pafupi nayenze Hattush mwana wa Hasabneiah anakonza. ¹¹ Malkijah mwana mwamuna wa Harimu na Hasshub mwana wa Pahati-Mowabu anakonza gawo inangu mosatira tawa yama fanasi. ¹² Pafupi nabenze Shallamu mwana wa Halloheshe, woyanganila hafu ya disitilikiti ya Yelusalemu, anakonza, mosatira naba nake bakazi. ¹³ Hanun na bonkala mu Zanoah banakonza chipata cha chigwa. Banayimanya nafuti nakufaka chiseko, nama bawuti, namipiringizo. Banakonza mikono il chikwi kufikila chipata cha ndowe. ¹⁴ Malkijah mwana wa Recabu, woyanganila na disitilikiti ya Beti Haeremu anakonza chipata cha ndowe. Anayimanga nakuyika chiseko, nama bawuti, namipiringizo. ¹⁵ Shalumu mwana wa Kol-Hozehe, woyanganila madilisilikiti ya Mizpa, anamanga nafuti chipata chakasupe. Anayimanga, nakuyika chivinnikolo pamwamba nakuyika chiseko, ma bawuti, namipiringizo. Anamanga nafuti khoma ya dziwe ya Silomu mu munda wa mfumu, kufikila ku masitepe yeyanda pansi kuchokela mu muzinda wa Davide. ¹⁶ Nehemiya mwana wa Azbuki, woyanganila theka ya disilikiti ya Beti Za, anaonza kufika kumalo yopila kuchokela ku manda ya Davide, kufika kudziwe yopangiwa na bantu, naku nyumba ya bamuna bampamvu. ¹⁷ Kuchokela enve ba Levayiti banakonza, kufikilapo Rehumu mwana wa Bani nakufupi nayenze. Hashabayi, woyanganila theka ya disitilikiti ya Keila, ku disilikiti yake. ¹⁸ Kuchokela yenve ba bale bawo banakonza, kufakikapo Binnui mwana wa Henadadi, woyanganila theka ya disilikiti ya Keilah. ¹⁹ Pafupi nayenze, Ezeri mwana wa Yesua, woyanganila pali Mizpa, anakonza gawo inangu yamene inali kuyangana kukwera kuzida zankondo pa ngodya ya chibumba. ²⁰ Kuchokela enve Baruchi mwana wa Zabbai mwachangu anakonza gawo inangu, kuchokela ku ngodya ya chibumba kufikila chiseko chanyumba ya Elishibi mukulu wansembe. ²¹ Kochokela enve Meremoth mwana wa Uriah mwana wa Hajjozi anakonza gawo inangu, kuchokela kuchiseko chanyumba ya Eliashib kufikila kosilila nyumba ya Eliashib. ²² Pafupi nayenze bansembe, bamuna bamu malo yozinguluka Yelusalemu, banakonza. Kochokela benve Benjamin na Hasshub banakonza moyanganizana nyumba yabo. ²³ Kochokela benve Azariya mwana wa Maaseiah mwana wa Ananiah anakonza pafupi na nyumba yake. ²⁴ Kochokela yenve Binnui mwana wa Henadadi anakonza gawo inangu, Kochokela ku nyumba ya Azariya kufikila kungodya ya chibumba. ²⁵ Palali mwana wa Uzai anakonza moyanganizana ngodya yachibumba na tawa yamene iyendeleda kumwamba kuchokela kunyumba yapamwamba ya mfumu pa bwalo yabamalonda. Kochokela yenve pedaya mwana wa Parosh anakonza. ²⁶ Manje bakapolo bamu tempele bonkala mu Ophel banakonza kufikila kumalo yoyanganizana chipata cha manzi chakumawa na tawa yochokelela. ²⁷ Kochokela yenve ba Tekoyiti banakona gawo inangu, yamene inali yoyanganizana a tawa ikulu inali yochokelela kufikila kuchibumba cha Ophel. ²⁸ Bansembe banakonza pamwamba pa chipata cha kavalo, alionse kuyanganiza nanyumba yake. ²⁹ kukonka benve Zadoki mwana wa immer anakonka gawo yoyanganiza nyumba yake, Ndipo kukonka yenve Shemaya mwana wa Shecaniah, wosunga chiptata chakumawa, anakonza. ³⁰ Kukonka yenve Hananiah mwana wa Shelemiah, na Hanun mwana wa sikisi wa Zalaph, anakonza gawo inangu. Kukonka yenve Meshullamu mwana wa Berechiah anakonza moyanganiza chipinda chake chogona. ³¹ Kukonka yenve Malkijah, omwe wabo wosula golide, anakonza kufika ku nyumba ya kapolo wamu tempele na malonda yanali moyanganiza chipata cha musonkano na chipinda chogonela chapa mwamba pangodya. ³² Bo wosula golide na malonda banakonza pakarti pa chioinda chogona chapa mwamba cha ngodya na chipata cha nkosa.

Chapter 4

¹ Manje pamene Sanballati ananvela tinali kumanaga chibumba, anayaka mukati mwake, ndipo anankala wokwiya maningi, ananyioza ba Yuda. ² Pamenso ya abale bake nabankondo ba Samaria, anakamba kuti, "Nanga aba ba Yuda bofooka bachi dani? Bushe bazabwezesa muzinda kuli benve? Bushe bazapeleka Zopereka? Bushe zasasiliza nchito musiku imozi? Bushe babwelesa umoyo kumyala kuchokela ku milu ya zinyalala kuchokela kuviwocha?" ³ Tobiya muAmonayiti anali na enve, ndipo anakamba kuti, "ngati ngandwe yamkwela pamwamba pali vamene bali kumanaga, inga pwanje pansi chibumba chawa chamyala!" ⁴ Nvelani. Mulungu watu, ndise bonyozedwa. Bwezani kunyozzi kwawo pa mitu yawo nakubapereka kuti bankala bo funka mu malo yaupapolo. ⁵ Musavinikile kusaweruzika ndipo musankale machimo yawo kufufutiwa kuchokela pamenso panu, chifukwa bakwiyisa bomanga. ⁶ Tinamanga chibumba ndipo zibumba zonse zenze zolumikizikwa pamozi kupanga theka lakutipa kwayenve, chifukwa bantu banalikufunsisisa kusebenza. ⁷ Koma pamene Sanballati, Tobiya, ba Alabiyani, ba Ammonayiti, naba Ashdodayiti bananvela kuti nchito yakukonza vibumba va Yelusalemu inali kuyenda pasogolo, nakuta mali yowanyika muchibumba yanalikuvaliwa, nkiyo ikulu inayaka mukati mwawo. ⁸ Bonse banapanga pamozi, ndipo banabwela kumenyana na Yelusalemu nakuleta musokonezo. ⁹ Koma tina mpepela kuli mulungu watu ndipo anayika malonda wotuteteza kuli benve muzuba nausiku chafukwa chakuosezza kwawo. ¹⁰ Ndipo bantu ba Yuda banakamba kuti, "Mpavu za baja bonyamula cholemesa zalephela. Kuli zinyalala za mbili, ndipo sitikwanisa kumanga chibumba nafuti." ¹¹ Badani batu banakoambakuti, "Sibazaziba nangu kuwona kufikila tufike pakati kawo naku ba paya, nakulekeza nchtio." ¹² Panrawi ija ba Yuda bamene banali kunkala pafupi na benve banabwela kuchokela mbali zonse nakukumba nayise kwantawi zili teni, kutichenjeza pali chiwembu chamene banali kupangila ise. ¹³ Ndipo ninayika bantu mu mbali za pansi zachibumba mumalo yamene siyobisika. Ninayika banja iliyonse nama panha yawo, mkondo, na mauta. ¹⁴ Ninayangana, nkunyamuka, ndipo ninakamba kuti kuli bolemeseka, nakuli bolamulila, naku bantu bonse, Musabayope. itanani munzeli Mulungu, wamene ali wamkulu, wodabwisa. Menyelani ma banja yanu, bana banu bamua naba kazi, bakazi banu, nama nyumba yanu." ¹⁵ Inafika pamene badani batu bana nvela kuti mapulani yabo tiyaziba, ndipo Mulungu anakumudwisa mapulani yabo, ise bonse tinabwelela kuchibumba, aliyense ku nchito yake. ¹⁶ Kuchokela pantawi ija theka yaba kapolo banga baa sebenzela chabe paku manga chibumba nafuti, ndipo theka yabenangu inagwila mkondo, chisongo, mauta nakuvala zida zankondo, pamene ba sogoleli banayimilila kumbuyo kwa bantu bonse ba Yuda. ¹⁷ Ndipo baja banali kumanga chibumba. Baja banali kunyamula chilimezo bananyamula njila zawo chakuti aliyense anachita nchito yake nakwanja kumoi, ndipo na kwanja kwinangu ananyamula chida. ¹⁸ Womanga aliyense ananvela panga yake yomangiwa pambali pake, ndipo ndiye mwamene anasebenzela. Bamene bana zunguluka lipenga anankala pambali pake. ¹⁹ Ninakamba kuti kuli bolemeseka nakuli boyanganilia naku bantu bonse, "Nchito nikulu komonso ikulu, ndipo ndise ikanisidwa pachibumba, kutali namuzanke. ²⁰ Mufunika kutamangila kumalo kwamene munvela fokoso yalipenga naku sonkana kuja. mulungu watu azatimenyela." ²¹ Ndipo teze kuchita nchito, theka la benve banali kugwila mkondo kuchokela kutuluka mbanda kucha kufikila paku chokela kwa nyenyezi. ²² Naine ninakamba kubantu pantawi ija, "Lekani mwamu aliyense nan kapolo wake ankale usiku mukati mwa Yelusalemu, chakuti bankale ba malonda batu usiku nakunkala banchito muzuba." ²³ Koteri, kapena abale banga, kapena bakapolo banga, kapena bamuna bamalonda bamene bananikonka, palibe aliyense wa ife amene anachinja zovala, ndipo aliyense wa ife anayamula chida, ngakale atapita kokatunga manzi.

Chapter 5

¹ Ndipo bantu na bakazi banyamu kulila kwachikulu mosusana ba Yuda bazawo. ² Chifukwa kunali benangu banali kukamba kuti, "Na bana batu bamuna naba kai tili bambili. Tiyeni titenge tirigu kuti tidye nakunkala wa moyo." ³ Kunali benangu nafuti bana kamba kuti, "Tikongolesa minda yatu, mind yampesa, na manyumba yatu kuti titenge tirigu muntawi yanjala." ⁴ Benangu banakamba kuti nafuti, "Takongola ndalama kulipila musonko wanfumu pa minda yau na minda yampasa." ⁵ Koma manje tupi latu na gaz niyimozi naya abal batu, ndipo bana batu nibamozi bawo. Takakamizidwa kugulisa bana batu bamuna naba kazi kunkala bakapolo. Bana batu bakazi benangu niba kapolo kudala. Koma sizili mumpavu zatu kutandiza chifukwa bamuna benangu manje bali na minda zampesa yatu." ⁶ Ninakalipa pamene ninavela kulila kwawo na mawu aya. ⁷ Ndipo ninaganiza pal ichi, naku chita upilo wampavu kuli bolemekezeka nabo yanganila. Ninakamba kuti kuli benve, "mufuna chiwongola zanja, aliyense kuchokela kuli bale wake" ⁸ nakumba kuli benve, "Kuli ise, tili nazo. kulinga na mpamvu zatu, tinagwa nafuti kuchokela ku ukapolo able atu ba Yuda bamene benze bana gulisiwa ku chalo, koma munagulisa able banu chakuti bagulisiwe kuli ise!" bankale chete ndipo sibanapezekenamawo yo kamba. ⁹ Naafuti ninakamba, "Vamene muchita sivabwino. Simuyenda kuyenda mukuyopa Mulungu watu kupwea bonyoza bamu chalo bamene bali niba dani batu?" ¹⁰ Ine na abale banga na kapolo banga tibakongolesa ndalama na tiligu. Koma tifunika kusiya kulipilisa chiwongola zanja pa nkongole izi. ¹¹ Bwezani kuli benve lelo yamene minda yawo, minda yampesa, munda wa azitona, manyumba yabwo na kuchuluka kwa ndalama, tiligu, vinyu yasopano namafut yamene munafuna kuli benve." ¹² Ndipo banakamba kuti, "Tizabweza zamene tinatenga kuli benve, sitizafuna nachilichonse kuchokela kuli benve. Tizachita zamene watiwuza." Ndipo ninayitana ansembe, naku balumbilisa kuti bachite zamerne bana lonjeza. ¹³ Nina nyan'anyisa mwnjiro yanga nakukamba kuti, "Mulungu anayang'nyise kuchokela munyumba mwake na katundu ya muntu aliyense wamene sazasunga lonjezo yake. Chakuti anyang'nyisiwe naku kesedwa." Bonse bolongana banakamba kuti, "Ameni," Ndipo banatamanda Yehova ndip bantu banachita zamene bana lonjeza. ¹⁴ Kochokela ntawi yamene ninansankiwa kunkala kazembe wabo mualo ya Yuda, kuchokela mumwaka wa twenti kufikila mumwaka wa sate-tu wa Artaxerxes mfumu, myika twelufu, ngakale ine kapena abale banga chokudya chopasiwa kuli kazembe. ¹⁵ Koma bakazembe bakale banaliko banayika zolemesa zikulu pa bantu, nakutnga kuli benve masekeli ya siliva ya fote kuckela kuli zokudya zawo na vinyu. nabakapolo babo banali mfumu pa bantu. Koma sinachite ivi chifukwa chakuyopa Mulungu. ¹⁶ Naine ninakonkaya kusebenza pachibumba, ndipo sitina gila malo, ndipo bonse bakapolo banga banankala pamozi pa nchito. ¹⁷ Pa tebulo yanga kunali ba Yuda yangila bawo, bamuna bali 150, kuchosela baja banabwela kuli ise kuchokela mukati mwachalio chenzo tizignuluka. ¹⁸ Manje zamene zenza pangiwa masiku yonse inali ng'om e imozi, nkosa zili sikisi, na zinyoni, mumasiku yonse yali teni mitundu yonse ya vinyu inali yambali, koma kuli ivi vonse sinina oindeko gawo lazakudya kuli kazembe, chifukwa nchito inali yolema pa bantu. ¹⁹ Nitaneni munzelu, Mulungu wanga, bali zabwino, chifukwa chazamene nachitlia bantu aba.

Chapter 6

¹ Manje pamene Saballati, Tobiah, na Geshemu mu Arabu naba dani batu bonse bananvela kuti na manga nafuti chibumba ndipo kunalibe gawo iliyonse inasala yoseguka, ngakale sinenze nayika ziseko muzipata, ² Sanballati na Geshemu banatumila ine nakukamba kuti, "Bwela, tiyeni tukumane pamozi mumalo yalibe kali konse ya Ono." Koma banali kufuna kuchita zoyipa kuli ine. ³ Ninatuma utenga kuli benve, nokamba kuti, "Nichiya nchito ikulu, ndipo siningabwele pansi. Nichani chito iyimilile nikachoka nakubwela pal kuli imwe?" ⁴ Bananatumila utenga wamene kwantawi zi 4, ndipo nibayanka mwamene ntawi iliyonse. ⁵ Sanballati anatuma kapolo wake kuli ine munjila yamene ntawi ya 5, nankalata yoseguka mumanja mwake. ⁶ Mukati yenze yolembewa, Ine "Nichokambiwa pakati ka chalo, na Geshemu nayenve akamba kuti, iwe naba Yuda mupulana ku panduka, ndiye chamene mumangila chibumba. Kuchoka mwamene malipoti akamba, iwe ufuna kunka mfumu yawo. ⁷ Wasanka baneneli kuti bapange ichi chilingezo mu Jerusalemu, kukamba kuti, "kuli mfumu mu Yuda! Ungakale wosimikize mfumu aza nvela malipoti aya. Choncho bwela, tiyeni tikambe kani iyi pamozi." ⁸ Ndipo ninatuma mwau kuli enve kukamba kuti, "kulibe zintu zachichitika mwamene ukambila, chifukwa wavipangila mumutima wako." ⁹ Chifukwa bonse banali kufuna kuti ise tiyope benzoganiza, "manja yawo yazasiya nchito, ndipo nchtio sizachitika." Koma manje, Mulungu, Napapata limbisani manja yanga. ¹⁰ Ninayenda kunyumba ya Shamaya mwana wa Delaya mwana wa Mehetabeli, anali wosekeledwa munyumba mwake, "Tiyene tikumane pamozi munyumba ya Mulungu, mukati mwa tempele, ndipo tivale viseko va tempele, chifukwa ba bwela kukupaya. Usiku babwela kukupaya." ¹¹ Nina yanka, "Nanga mwanuna alimonga ine angatabe? nanga mwamuna ali monga ine unga mu tempele kuti apulumuse umyo wake? Siniyenda mukati!" ¹² Ninazindikila sana tumiwe na Mulungu, koma anali kunenela kusuna Ine. Tobiya na Sanaballati benze mugula. ¹³ Bana mugula kuti aniyofye, chakuti nichite vamene anakamba naku chimwa, chakuti banapase zina loyipa kuti anchite. ¹⁴ Itanani munzeli Tobiya na Sanaballati, Mulungu wanga kukonya namachitidwe yawo. Muyitane munzeli na muneneli Noadiya na bonse bannenli beanyesa kuniyofya. ¹⁵ Chibumba chinasila pa sika la twenti faivi mumwezi wa Eluli, patapita masiku yali fifite tu. ¹⁶ Pamene ba dani bonse bananvela, maziko yonse yanaliku kuti zunguluka, banayopa nakugwa maningi pamenso yawo. Chifukwa banali kuziba kuti nchito inachitwa nama tandizo ya Mulungu. ¹⁷ Pantawi iyi bolemekezewa ba Yuda banatuma nkalata kuli Tobuya, naba nkalata ya Tobiya yanabwela kuli benve. ¹⁸ Chifukwa banali bambili mu Yuda banali bo mangiwa na lumbiro kuli enve, chifukwa anali mupongozi mwamuna wa Shekaniya mwana wa Arah. ¹⁹ Mwana wake Jehohanani enzeli anatenga mukazi wokwatila mwana wa Meshulam mwana wa Berechaya. Nabenve bananiwuzwa machitidwe yake yamushe nakuchita lipoti mawu yanga kuli yenvee. Nkalata zinatumiwa kuli ine kuchokela kuli Yobiya kuti aniyofye.

Chapter 7

¹ Mulungu wamene nimatamanda, Musa nkale zee ² Pakuti oipa na wachinyengo bani ukila; bani nenela va boza. ³ Bani zinga na ku kamba vintu vo voipa, ndipo amani ukila kulibe chifukwa. ⁴ Chifukwa cha chikondi changa bani nenela ine, koma ine niba pempelela. ⁵ Amani bwezela voipa mu malo mwa vabwino, ndipo bamani zonda chifukwa cha chikondi changa. ⁶ Ikani muntu oipa pa badani kwati aba bantu; ikani oneneza baime kuzanja yake lamanja. ⁷ Baka weluziwa, bapezeka olakwa; pempelo yake inkale yo chimwa. ⁸ Masiku yako ya nkale yagono;w ⁹ ^{10 11} Wa nkongole atenge vonse ali navo; bantu bosa zibika ba ononge vo kolola na manja yake. ¹² Pasankale ali yense omu chitila chifundo; pasankala winangu onvelela chisono bana bake bamasiye. ¹³ Bo badwa bake ba duliwe; zina yao ifafaniziwe mumbadwo osatila. ¹⁴ Machimo ya makolo bake yakumbukiliwe kwa Yehova; ndipo chimo ya bamai bake yasa ibalike. ¹⁵ Ma chimo yao yankale pa menso pa Yehova ntawi yonse; Yehova afafanize chikumbukilo chao pa ziko yapansi. ¹⁶ Yehova achite vamene ivi, chifukwa muntu bwa mene uyu sana vutikepo ku sonyeza chikulupilo olo pangono, koma mu malo mwake ana vutisa bantu opondelezewa, ovutika, na otaya mutima mpaka infu. ¹⁷ Eve ana konda kutembelela;lola izo zibwelele pa eve. Eve zonda daliso; dalitso izankale kutali na eve. ¹⁸ Anavala tembelelo kwati chovala chake, ndipo tembelelo yake ina ngena mukati mwake kwati manzi, kwati mafuta muma fupa yake. ¹⁹ Matembelelo yake yankale kwati vovala vamene ama vala kuzi vimba, kwati lamba yemene amavala ntawi zonse. ²⁰ Vamene ivi vinkale mpoto va odineneza yochokela kuli Yehova, amene amani kambapo voipa. ²¹ Yehova, Ambuye wanga, muni chitile ine chifundo chifukwa cha zina yanu. Pakuti chipangano chanu nicha bwino, ni pulumiseni. ²² Pakuti na sausiwa na umpawi, ndipo mutima wanga walasiwa mukati mwanga. ²³ Ni silila kwati mtunzi wa mazulo; Na gwesewa kwati zombe. ²⁴ Nkonkola yanga ya foka na kosadya; tupi yanga ya yonda naku nkala kulibe mafupa. ²⁵ Nina nkala chintu cho nenewa; baka niona, bama nyanga nyisa mitu yao. ²⁶ Ni tandizeni, Yehova Mulungu wanga; ni pulumuseni na chipangano chanu chokulupilika. ²⁷ Bazibe kuti ndimwe munachita ivi, kuti imwe Yehova, mwachita ivi vintu. ²⁸ Okuti bani tembelela, mumani dalisa; akani ukila, bachitiwe manyazi, koma mutumiki wanu akondwele. ²⁹ Ba dani banga ba nvale manyazi; banvale manyazi nabeve kwati mwinjilo. ³⁰ Niza yamika Yehova kwambili na pakamwa panga; Niza mutamanda pakati pa bantu. ³¹ Pakuti azaimilila ku kwanja yamanja ya osoba, kuti amu pulumuse kuli bamene omu weluza.

Chapter 110

¹ Yehova ana kamba kuli Mulungu kuti : " Nkalani ku kwanja yanga lamanja mpaka ni pange adani banu cho dyakapo mendo yanu. " ² Yehova aza tambasula ku Ziyoni ndodo ya mpamvu yako; lamulilani pakati pa adani banu. ³ Bantu bako bazaku konka baka nvela voyela mukufuna kwao pa siku ya mpamvu yako; kuyambila mu mimba mwa mubandakucha ubwana wako uza nkala kuli iwe kwati mame. ⁴ Yehova alumbila ndipo saza chinja maganizo yake; " Iwe ndiwe wansembe kosata monga mwa chilongosolewe cha Melekizedeki. ⁵ Ambuye ali pa kwanja yako yamanja. Eve aza paya ma mfumu pa siku ya ku kalipa kwake. ⁶ Iye aza weluza ba mitundu; aza zulisa mabwalo ya nkondo na tupi za okufa; aza paya ba sogoleli ba maziko yambili. ⁷ Aza mwa manzi ya mu musinje ya mu mpepete mwa njila, ndipo kenako aza chosa mutu wake akapambana.

Chapter 111

¹ Tamandani Yehova. Niza yamika Yehova na mutima wanga onse pa musonkano bwa bo ongoka mutima, pa kusunkana kwabo. ² Nchito ya Yehova ni ikulu, ndipo aliyense wamene ama zilakalaka ali kuyemekezela mwa chidwi. ³ Nchito yake ni yolemekezeka na yolemekezeka, ndipo chilungamo chake chiza nkalapo mpaka muyaya. ⁴ Amachita vodabwisa vamene viza kumbukiliwa; Yehova ni wachisomo na cifundo. ⁵ Ama pasa chakudya kuli osatila bake okulupilika. Ntawi zonse aza kumbukila pangano yake. ⁶ Ana langiza nchito zake za mpamvu kuli bantu bake poba pasa cholowa cha mitundu. ⁷ Nchito ya manja yake nizo dalilika na zolungama; malangizo yake yonse ni yodalilika. ⁸ Ama nkazikisiwa kosata, kuti bazi onewa mo kulupilika na moyenela. ⁹ Ana peleka chipulumuso kuli bantu bake; ana nkazikisa chipangano chake kosata; zina yake ni yoyela na ku wama. ¹⁰ Kulemekeza Yehova ni chiyambi cha nzelu; bamene ama satila malangizo yake ama mvesesa bwino. Matamando yake yama nkala kosata.

Chapter 112

¹ Tamandani Yehova. Odala ni muntu wamene amayopa Yehova, wamene ama kondwela kwambili na malamulo yake. ² Bana bake baza nkala ba mpamvu pa ziko yapansi; bana ba muntu olungama baza dalisiwa. ³ Mu nyumba mwake muli chuma na chuma; chilungamo chake chiza nkala chosata. ⁴ Ku onika kuma walila mu mudima kuli muntu opembeza; na wachisomo, wachifundo, na olungama. ⁵ Zima nkala bwino kuli muntu bwamene amachita vintu mwa chifundo na ku bwelekesa ndalama, wamene amachita vintu vake moona mutima. ⁶ Pakuti Eve saza gwedezeka ku ntawi zonse; olungama aza kumbukiliwa kosatha. ⁷ Sa yopa mbili yoipa; akulupilila Yehova; ⁸ Mutima yake ili bata, opanda manta, mpaka ayangana mo pambana badani bake. ⁹ Apasa osauka mowolowa manja; chilungamo chake chinkale chosata; baza kwezewa na ulemu. ¹⁰ Oipa bazaona ivi vintu na ku kalipa; baza kokota meno na ukali naku sungunuka; zo funa bantu boipa viza taika.

Chapter 113

¹ Tamandani Yehova. Mulemekezeni, imwe atumiki ba Yehova; lemekezani zina ya Yehova. ² Zina ya Yehova idalisike, kuyambila manje mpaka muyayaya. ³ Kuyambila ko chokela zuba kufikila ko ngenela zuba, zina ya Yehova iyenela ku tamandiwa. ⁴ Yehova wakwezewa pamwamba pa mitundu yonse, na ulemelelo wake ufikila tambo. ⁵ Ndani ali moonga Yehova Mulungu watu, wamene a nkala mu mupando wake kumwamba, ⁶ wamene ayangana kumwamba na ziko yapansi? ⁷ Eve amausha wosauka mu doti naku kweza osauka ku muchosa pulusa, ⁸ kuti amu nkazike pamozi na akalonga, na akalonga ba bantu bake. ⁹ Apasa nyumba mukazi osabala wa mu nyumba; amu panga eve ku nkala mai wa bana bokondwa. Tamandani Yehova!

Chapter 114

¹ Pamene Israyeli anachoka mu Igupto, nyumba ya Yakobo kuchokela kuli bantu okamba chinenelo chacilendo, ² Yuda ana nkala malo yake yoyela, Israyeli ufumu wake. ³ Nyanja inayangana naku taba; Yordano ina tembenuka. ⁴ Mapili yana jumpa kwati nkosa za mpongo, vitunda vina jumpa kwati bana ba nkosa. ⁵ Watabila chani nyanja iwe? Yordani, yabwelela chifukwa chani? ⁶ Mapili, wa jumpa bwanji kwati nkosa zampongo? Imwe mapili, mujumpa bwanji kwati bana ba nkosa? ⁷ njenjeme, ziko yapansi, pa menso pa Yehova, pa menso pa Mulungu wa Yakobo. ⁸ Bana sandusa mwala ku nkala tamanda ya manzi, mwala yolimba ku nkala kasupe wa manzi.

Chapter 115

¹ Osati kuli ise, Yehova, kwa ise, koma kuli zina yanu lemekezani, chifukwa cha ku kulupilika kwanu na ku kulupilika kwanu. ² Aza nenanji bamitundu, "Ali kuti Mulungu wabo?" ³ Mulungu watu ali ku mwamba; amachita chilichonse chimene afuna. ⁴ Mafano ya bamitundu ni siliva na golidi, nhcito ya manja ya bantu. ⁵ Mafano yamene ayo yali na pakamwa, koma siya kamba; menso yali nayo, koma siya ona, ⁶ matu yali nayo, koma siya mvela; yali na mpuno, koma siya nunshsa. ⁷ Mafano ayo yali na manja, koma siya gwila; mendo yali nayo, koma siya ma yenda; na futi siya kamba vo tuluka mu kamwa yao. ⁸ Bamene bama zipanga afanana nao, monga aliyense ozikulupilila. ⁹ Israyeli, kulupilila Yehova; ndiye tandizo yako na chikopa chako. ¹⁰ Imwe ba nyumba ya Aroni, kulupililani Yehova; ndiye tandizo yako na chikopa chako. ¹¹ Imwe bamene muma lemekeza Yehova, kulupililani eve; ndiye tandizo yako na chikopa chako. ¹² Yehova ama tisamalila ndipo azati dalisa; aza dalisa banja ya Israyeli; aza dalisa banja ya Aroni. ¹³ Eve aza dalisa bamene bama mulemekeza, bana na bakulu. ¹⁴ Yehova aculukise chiwelengelo chanu, imwe na bazikulu banu. ¹⁵ Adalise Yehova wamene ana lenga kumwamba na ziko ya pansi. ¹⁶ Kumwamba nikwa Yehova; koma ziko yapansi anapasa bantu. ¹⁷ Okufa salemekeza Yehova, olo ali yense onkala chete; ¹⁸ Koma tiza tamanda Yehova sopano mpaka muyayaya. Tamandani Yehova.

Chapter 120

Nyimbo yokwezekela. ¹ Mumasauso yanga ninaitana kuli Yehova, ndipo ananiyanka. ² Pulumusani umoyo wanga, Yehova, kuchokela kuli bamene bama nama boza namilomo zao naku nama na malilime yao. ³ Nanga azakulangani bwanji, ndipo azakuchitila chani futi, iwe wamene uli na lulimi yonama? ⁴ Azakulanga na mivi ya musilikali yonolewa pamulilo wankuni. ⁵ Wasoka ndine chifukwa sinimankalisa mu Meshechi; kudala ninankala pakati pa mahema ya Kedara. ⁶ Kwa ntawi itali nankala na abo bamene sibakonda mutendele. ⁷ Ndine wamutendele, koma nikakamba, niba nkondo.

Chapter 121

¹ Nyimbo yokwezeka. nizakweza menso yanga kumapili; Tandizo yanga izachokela kuti? ² Tandizo yanga ichokela kuli Yehova, wamene anapanga kumwamba na ziko lapansi. ³ Sazavomeleza kwendo yako kushalemuka; iye wamene amakuchingiliza sazakusila. ⁴ Ona, woyanganila Israeli sakusila kapena kugona. ⁵ Yehova ndiye okuyanganilani; Yehova ndiye mutunzi ku kwanja yako yamanja. ⁶ zuba sizaku ocha muzuba, ngankale mwezi usiku. ⁷ Yehova azakuchingiliza kuchokela ku zoipa zonse, ndipo azachingiliza umoyo wako. ⁸ Yehova azakuchingiliza muli vonse vamene uchita manje namuyayaya.

Chapter 122

¹ Nyimbo yokwezeka, ya Davide. Ninakondwela pamene bananiuza kuti, "Tiyeni ku nyumba ya Yehova." ² Yerusalemu, mendo yatu yaimilila pakati pongenela! ³ Yerusalemu, yomangiwa ngati muzinda okonzekewa bwino bwino! ⁴ Mitundu zikwela kufika ku Yerusalemu - mitundu za Yehova- ngati umboni wa Israel, kupeleka matamanda kuli zina ya Yehova. ⁵ Mipando yao yachiweluzo inaikiwa, mipando ya nyumba ya Davide. ⁶ Pempelelani mutendere wa Yerusalemu! "Lekani abo bamene bakukondani bankale na mutendele. ⁷ Lekani munkale mutendele mukati mwa vipupa vamene viku tetezani, ndipo lekani bankale namutendele mukati mwama linga yanu." ⁸ Chifukwa cha babale banga na banzanga nizakamba ati, "Mutendele unkale muli imwe." ⁹ Chifukwa cha nyumba ya Yehova Mulungu watu, nizakufunilani vabwino.

Chapter 123

¹ Nyimbo yokwezeka. Nikweza menso yanga kuli imwe, imwe onkazikisiwa mumwamba. ² Onani, monga menso ya wanchito yayanga kumanja yabwana wake, apenyera dzanja la mbuye wao, monga maso a mdzakazi ayang'ana dzanja la mbuye wace, momwemo maso athu ayang'ana kwa Yehova Mulungu wathu, kufikira aticitile cifundo. ³ Tichitleni chifundo, Yehova, timveleni chifundo, pakuti tazuliwa na manyazi. ⁴ Ndise bozula na manyozo ya bachipongwe na minyozo pa bozimvela.

Chapter 124

¹ Nyimbo yokwela; wa Davide. Yehova akaleka kunkala na ise, Israyeli akambe manje, ² Yehova akaleka kunkala na ise, pamene bantu banatiukila, ³ sembe anatemela tili bamoyo, pamene mkwiyo wao unatikwiya. . ⁴ Manzi sembe yanatipya; mimana yamene iyi; sembe inatitika. ⁵ Sembe yanatemela manzi yoyofya yamene aya." ⁶ Atamandike Yehova, wamene sanatikelele kuti bating'ambe ng'ambe na meno yao. ⁷ Tapulumuka munga mbalame mumsampa wa bogwila nsomba; msampa wa tyoka, ndipo tapulumuka. ⁸ Tandizo yatu ili muli Yehova, wamene analenga kumwamba na ziko yapansi.

Chapter 125

² Nyimbo yokwela. ¹ Bokulupilila Yehova bali monga pili ya Ziyoni, yosagwendezeke, yonkazikika kwamuyayaya. 2 Monga mapili yozunguluka Yerusalemu, ndiye mwamene Yehova azungulukila bantu bake manje na muyayaya. ³ Nkoli dodo yauchimo siyenela kulamulila muziko ya bolungama. Ngati si ivo bolungama bangachite Choyipa. ⁴ Imwe Yehova, chitolani vabwino bantu babwino na bo ongoka mtima. ⁵ Koma beve bamene iwo amene batembenukila ku njila zao zosalungama, Yehova azaatsogolela pamozi na bochita voipa. Mtendele unkale pali Israyeli.

Chapter 126

¹ 1Pamene Yehova anabweza bogwiliwa a Ziyoni, tezenli baja bolota ² Pamenepo mukamwa mwatu munazaza nakuseka na lulime yatu na kuimba kwachikondwelelo. Pamene anakamba kuli bamitundu, Yehova abachitira vikulu; ³ Yehova anaticitila ife vikulu; tinali okondwa bwanji nanga! ⁴ Bwezani bankondo bantu, Yehova, monga mumana ya ku Negebu. ⁵ Boshanga na mumisozi bazakolola na nakupunda kwa chikondwelelo ⁶ Iye wamene ayenda olila , anayamula mbewu nshanga, azabwelanso na kupunda kwachisangalalo, poleta vokolola vao mu nyumba pa ntawi yavokolola.

Chapter 127

¹ Kano Yehova amanga nyumba,basebenza pachabe chabe ,baja bo manga. Koapanda Yehova kusunga muzi, malonda yalonda palibelibe . ² Nikwachabechabe kuti uuke kuseniseni, nakubwela mochedwa ku nyumba, kapena kuti udye chakudya chogwila nchito yampamvu , pakuti Yehova apasa chakudya kuli okondedwa bake pamene ba gona. ³ Onani,bana ni cholandila kuchokela kuli Yehova, na chipaso cha mumimba ni mpotho yochokela kuli eve. ⁴ Monga mivi mumanja ya muntu wankondo, monga bana bauchifana baumoji ⁵ . Odalisiwa muntu wamene ali navo vojenjemela vambili. Eve sazachita manyazi akakumana na badani bake pachipata.

Chapter 128

¹ . Niodalisiwa aliyense wolemekeza Yehova, oyenda munjila yake. ² Vamene manja yanu yapereka, muzasangalala nazo; muzankala odalisiwa na wanzelu. ³ Mukazi wako azankala monga mpesa yobala zipaso munyumba mwako; bana bako bazankala monga vomela va azitona, pamene bankala panshi pozungulikila tebulo yako. ⁴ Inde, muntu wamene amalemekeza Yehova azadaliswa. ⁵ Yehova akudaliseni bali mu Ziyoni; muone ubwino wa Yerusalemu masiku yonse ya moyo wako. ⁶ Munkale na moyo kuti muwone bana ba bana banu. Mtendele unkale pa Israyeli.

Chapter 129

¹ “Kawirikawiri bankala boniukila kuchokela kubwana wanga,” leka Isiraeli ikambe . ² Ntawi zambili bama nkala boniukila kuyambila kuubwana wanga, koma sibananigojeze. ³ Bolima balima pamusana panga;banatalimpisa mizela zawo. ⁴ Yehova ndiye wolungama; adula ntambo za oipa.” ⁵ Bachitisiwa manyazi na kubwelela kumbuyo, bamene bazondaZiyoni. ⁶ Bankale monga mauzu yapakomo yamene yamafota yakalibe kukula ⁷ yamene siyanga pake mumanja mwa okolola kapena m’bokosi ya omanga mbewu. ⁸ Bamene bapitapo basa kambe kuti, “Madalitso ya Yehova yankale pali imwe, tikudalisani muzina ya Yehova.

Chapter 130

¹ Nililila mukati kuli imwe, Yehova. ² Ambuye, velani mau yanga; matu yanu yavesese kulila kwanga kwa chifundo. ³ Ngati imwe, Yehova, musunga machimo, Yehova, nidani anga imilile? ⁴ Koma kuli kukululukiwa kuli imwe, kuti tiyope imwe. ⁵ Niyembekeza Yehova, moyo wanga ulindila, ndipo namu mau yake nichiyembekezo changa. ⁶ Moyo wanga ulindila Yehova kuchila malonda oidilila kuti kuche. ⁷ Israyeli, chiyembekezo chili muli Yehova. Yehova ni wachifundo na chikukululukilo. ⁸ Ndiye azawombole Isiraeli ku machimo yake yonse.

Chapter 131

Nyimbo yokwela; wa Davide. ¹ Yehova, mutima wanga siwozithukumula , kapena manso yanga ozikuza. Niliba ziyembekezo zazikulu kwa ine neka kapena kudzidetsa nkhawa na zinthu zimene sizikundiposa. ² Zoona chabe, natontholesa na kutontholesa moyo wanga; monga mwana wolesewa na amai wake, umoyo wanga uli ngati mwana wolesewa mukati mwanga. ³ Israyeli, yembekeza Yehova manje na mpaka muyayaya.

Chapter 132

¹ Nyimbo yokwela. Yehova, chifukwa cha Davide, kumbukilani masauso yake yonse. ² Kumbukilani mwamene analumbilila Yehova, mwamene analumbilila Wamphamvu wa Yakobo. ³ Anakamba kuti, “Sinizangena muchi hema cha munyumba mwanga, kapena kulowa pabedi yanga, ⁴ sinizapasa manso yanga tulo kapena mpumulo ku zikope zanga ⁵ mpaka nikapeze malo ya Yehova, chihema cha Wamphamvu wa Yakobo.” ⁶ Onani, tinamvela ku Efrata; tinaupeza muminda ya Yaari. ⁷ Tizalowa muchihema cha Mulungu; tizalambila pa chopondapo pamendo yake. ⁸ Nyamukani, Yehova, ku mpumulo wanu, Imwe na likasa ya mphamvu yanu! ⁹ Bansembe banu bavale ungwilo; okhulupilika banu akambe mokondwela. ¹⁰ Chifukwa cha Davide mutumiki wanu, musapatuke kuli wozozedwa wanu mfumu. ¹¹ Yehova analumbilia Davide na lumbilo losimikizilika kuti sazabweza eve: “Nizaika umozi wa mbadwo wako pamupando wako wachifumu. ¹² Ngati bana bako basunga chipangano changa na malamulo yamene nizabaphunzisa, bana bonse bazankhala pamupando wako wachifumu wamuyayaya.” ¹³ Zoona Yehova wasanka Ziyoni, ndipo wamufuna kuti unkhale mupando wake. ¹⁴ “Apa ni malo yanga yopumulilamo mpaka muyayaya. Ndipo nizankhala pano, chifukwa nimamufuna.” ¹⁵ Nizamudalisa kwambili na chakudya. nizakhutisa bosauka bake na buledi. ¹⁶ Bansembe bake nizabavalika chipulumuso, okhulupilika bake azafuula mokondwela. ¹⁷ Kwamene uko nizameresanya nyanga ya Davide ndipo nizamuyashila nyali wozozedwa wanga. ¹⁸ Adani bake nizabavalika manyazi, koma korona wake izawala pali iye.

Chapter 133

¹ Nyimbo yokwela ya Davide. Onani, nichabwino na chokondwelesa kuti abale ankhale pamozi ! ² Zili ngati mafuta osalala pamutu otsikila pa ndevu- ndevu za Aroni, ndipo imatayikila pamphuno wa zovala zake. ³ Uli ngati mame Ya ku Hermoni yamene yamagwa pa mapili ya Ziyoni. Pakuti kwamene uko Yehova analamulila madaliso - umoyo wamuyayaya.

Chapter 134

¹ Nyimbo yokwela. Bwelani, lemekezani Yehova, iwe bonse atumiki ya Yehova, imwe bamene mukutumikila usiku munyumba ya Yehova. ² nyamulani manja yanu kumalo yoyela ndipo lemekezani Yehova. ³ Yehova akudaliseni kuchokela ku Ziyoni, wamene analenga kumwamba na ziko yapansi.

Chapter 135

¹ Tamandani Yehova! Lemekezani zina Ya Yehova. Mutamandeni eve, imwe atumiki ya Yehova, ² imwe bamene mumaimilila munyumba ya Yehova, mumabwalo ya nyumba ya Mulungu wathu. ³ Lemekezani Yehova, pakuti ndiye wabwino; imbani zotamanda zina yake, pakuti nichokondwelesa. ⁴ Pakuti Yehova asankha Yakobo kuti ankhale wake, Israeli ankhale chuma chake. ⁵ Niziba kuti Yehova ni wamukulu, kuti Ambuye wathu ni woposa milungu zonse. ⁶ Chilichonse chamene Yehova afuna amachichita kumwamba, paziko yapansi, munyanja na munyanja zonse zakuya. ⁷ Iye amabwelesa mitambo kuchokela kutali, kuchitisa mphezi kutsata mvula, na kutulusa mpempo munkhokwe yake. ⁸ Anapaya mwana oyamba kubadwa wa Aigupto, banthu na nyama. ⁹ Anatumiza zizindikilo na zodabwisa pakati pako, Aigupto, pa Farao na atumiki bake onse. ¹⁰ Anamenya mitundu yambili naku paya mafumu amphamvu, ¹¹ Sihoni mfumu ya Aamori, na Ogi mfumu ya Bashani nama ufumu onse ya Kanani. ¹² Anatipasa ziko yawo ngati cholowa, cholowa cha Aisiraeli banthu bake. ¹³ Zina yanu, Yehova, izankhalapo muyayaya; mbili yanu, Yehova, izankhalapo ku mibadwomibadwo. ¹⁴ Pakuti Yehova amateteza banthu bake ndipo amachitila chifundo atumiki bake. ¹⁵ Mafano ya mitundu ni siliva na golide, nchito ya manja ya banthu. ¹⁶ Mafano yali na makamwa, koma siyamakamba; manso yali nawo, koma siyamayangana; ¹⁷ matu yali nawo, koma siyamamvela, ndipo mukamwa mwao mulibe mpweya. ¹⁸ Bamene bapanga izi ali monga vamene ivi. monga onse wamene akhulupilila muli ivi. ¹⁹ Iwe bana ba Israyeli, lemekezani Yehova; mibadwo ya Aroni, lemekezani Yehova. ²⁰ Iwe a mbumba za Levi, lemekezani Yehova; imwe bamene amalemekeza Yehova, lemekezani Yehova. ²¹ Wolemekezeka Yehova mu Ziyoni, iwe wonkhala mu Yerusalemu. Tamandani Yehova.

Chapter 138

¹ Sailmo ya Davide. Nizakuyamikani ni mtima wanga onse; pameso pa tumilungu nizakuyimbilani mothokoza. ² Nizagwada nakuyangana Kachisi yanu yoyela, na kuyamika zina yanu chifukwa chapangano ya kukhulupilika na chilungamo chanu. Mwapanga mau yanu na zina yanu kukhala yofunika manigi kuchila chilichonse. ³ Siku yamene ninakuitanani, munaniyankha; munanipanga olimba ndipo munakosesa moyo wanga. ⁴ Mafumu yonse ya ziko yapansi yazakuyamikani, Yehova, pakuti yazamvela mau ochka pakamwa panu. ⁵ Inde, bazaimba va ntchito ya Yehova, pakuti ulemelelo wa Yehova ni ukulu. ⁶ Pakuti ngakhale Yehova ali okwezekewa, asalalila bapansi; Koma ozimvesa amazibila pali kutali. ⁷ Olo niyenda pakati pa voyofya, muzasunga moyo wanga; muzatambulula kwanja yanu mukali kuli badani banga, ndipo kwanja yanu yamanja izanipulumusa. ⁸ Yehova ali naine kufikila posilizila; chipangano chakukhulupilika kwanu, Yehova, kukhala muyayaya. Musaibale baja bamene manja yanu yanapanga.

Chapter 139

¹ Yehova, mwaniyesa, ndipo mwanizibaa; ² Muziba nika nkala pansi, na pamene na nyamuka; muziba maganizo yanga ya kutali. ³ Muma ona mayendedwe yanga naku gona kwanga; muziba njila zanga zonse. ⁴ Pakuti panga nkale mawu pa lulimi yanga, imwe muziba bwino, Yehova. ⁵ Kumbuyo kwanga na kale mumani zungulila na kufaka kwanja yanu pali ine. ⁶ Kuziwa kotele kwanichepela ine; nikwapa mwamba manigi, ndipo sininigafikepo . ⁷ Nizayenda kuti kuchokela pu Muzimu wanu? ningatabile kuti kuchokela pamenso panu? ⁸ Nikakwela kumwamba, muliko; nikapanga pogona panga kumanda, onani, muliko. ⁹ Nika mbululuka na mapepe kwakucha, nakuyenda ku nkala ku kwambili ku malekezelo ya mumana ukukulu ya manzi. ¹⁰ Nauko manja yanu yazanisogolela, manja yanu yazanigwila. ¹¹ Nika kamba , Ndipo mudima uzani vinikila, na kuunika kuza nkala usiku pozungulukila ine ¹² Nakufipa kuza nkala kufipa kuli imwe. Pakuti kufipa kuzawala monga muzuba, chifukwa kufipa nakuwala konse kuli monga chimozi kuli imwe. ¹³ Munapanga vamukati mwanga; munani panga mumimba mwa amayi banga. ¹⁴ Nizakutamandani chifukwa munanipanga moopsa na modabwisa. Ntchito zanu nizodabwisa. Moyo wanga uziba bwino izi. ¹⁵ Mafupa yanga siyanabisame kuli imwe, pamene ninapangiwa ndeka, pamene ninapangiwa movutikila pa ziko yapansi. ¹⁶ Munaniona mumimba; masiku yonse yamene ninapasiwa yanalembewa mubuku yanu, kale yoyamba ikalibe kuchitika ¹⁷ Maganizo yanu naya mutengo wapatali kuli ine, Mulungu! Ni kuchoka kwa bwanji! ¹⁸ Nikayesa kupenda, zingachile muchanga. Nikauka, nikali na imwe. ¹⁹ Ngati munga paye boipa, Mulungu; chokani pali ine, bantu botila magari imwe. ²⁰ Bamakupandamukila na kuchita boza; badani bako bamanama. ²¹ Kodi sinimaba zonda abo, Yehova, nidani akuzonda? Kodi sinimaba nzonda bamene bakuukila? ²² Nibazonda abo kumalizilatu; bama nkala badani banga. ²³ Muniyese ine, Mulungu, na kuziba mutima wanga; muniyese na kuziba maganizo yanga. ²⁴ Onani ngati muli njila yoipa muli ine, nakunisogolela njila yosata.

Chapter 140

Kuli woyimba mukulu. Salimo ya Davide. ¹ Yehova, nipulumuseni kuli boipa; nipulumuseni ku bantu bankanza. ² Bakonza voipa mumitima mwao; bamayambisa nkondo siku iliyonse. ³ Malilimi yao yalasa monga njoka; Ululu wa njoka uli pa milomo zao. Selah ⁴ Nisungeni mumanja mwa boipa, Yehova; nipulumuseni ku bantu bankanza bamene bafuna kunigwesa. ⁵ Bozikuza baniteyela musampa; bayanzika sumbu; baniteyela musampa. Selah ⁶ Ninakamba kuli Yehova, Imwe ndimwe Mulungu wanga; mvelani kulila kwanga; ⁷ Yehova, Ambuye wanga, ndimwe ba mpamvu bokwanisa kunipulumusa; Munichingiliza mutu wanga siku yankondo. ⁸ Yehova, musapase boipa vilako lako va mitima yao; musavomeleze misampa yao kufilikizika. Selah ⁹ Bamene banizungulila banyamula mitu yao; voipa va milomo yao vibavininkila. ¹⁰ Malasha yoyaka mulilo ubagwele; baponyeni mumulilo, mu nganjo ya moto, kuti basakaukepo futi. ¹¹ Bantu bamalulimi basatetezewa pa ziko ya pansi; choipa chibakonke kufika kuli muntu wankanza kuti amupaye. ¹² Niziba kuti Yehova azaweluza muchilungamo bovutika, nikamba kuti azaweluza bosauka. ¹³ Zoona bolungama bazayamikila zina yanu; bolungama bazankala pamenso panu.

Chapter 141

Salimo ya Davide. ¹ Yehova, nililila kuli imwe; bwelali kuli ine musanga. Munimvele ine pokuitanani. ² Pempelo yanga inkale monga vofukiza pamenso panu; manja yanga mumwamba monga nsembe ya kumazulo. ³ Yehova, ikani kamalonda pakamwa panga; sungani komo ya mulomo wanga. ⁴ Mutima wanga usakumbwe choipa chilichonse kapena kuchita nabo pamozi voipa bantu bochita voipa. Nisadyeko vambwino vao vilivonse. ⁵ Muntu wolungama animenya; chizankala chabwino kuli ine; Musiyeni anibweze ine; yazankala ngati mafuta pamutu panga; mutu wanga usakane kuyalandila koma pempelo yanga ntau zonse imashushana na voipa vao. ⁶ Basogoleli bao bazagwesewa kuchokela pamwamba pa vimyala vikulu ; bazamvela kuti mau yanga ni yokondwelesa. ⁷ beve bazakamba ati, “Monga mwamene muntu amalimila na kupwanya ntaka, ndiye mwamene mabonzo yatu yamwazyikilana pamulomo pa sheol. ⁸ Zoona, menso yanga yali pali Imwe, Yehova, Yehova; muli Imwe ndiye mwamene nitabila; musasiye umoyo wanga ninshi ulibe chonichingiliza. ⁹ Munichingilize ku misampa yamene bani ikila, Ku misampa ya bochita voipa. ¹⁰ lekani boyipa bagwele mumasumbu yao, ine nipulumuke.

Chapter 142

¹ Nyimbo ya Davide, pamene enze mu mpako; pempelo. Ndilirira mau anga kwa Yehova; na liwu yanga nipempa Yehova kuti aniwamile mutima. ² Nikutula kulila kwanga pamenso pake; Nimamuuza mavuto yanga. ³ Pamene muzimu wanga wafoka mukati mwanga, mumaziba njila yanga. Munjila yamene nimayendamo banibisila msampa. ⁴ Nimayangana kukwanja yanga yamanja ndipo nakuona kuti kulibe nawamene anisamala. kulibe na kotabila; kulibe na wamene asamalila pali umoyo wanga. ⁵ Ninabuula kuli imwe, Yehova; Ninakamba kuti, “Imwe ndimwe kotabila kwanga, mbali yanga muziko ya bamoyo. ⁶ Mvelani kuitana kwanga, pakuti nachepesewa; nipulumuseni mumanja ya bonisaua, pakuti banichila mpamvu. ⁷ Chosani umoyo wanga mu ndende kuti niyamike zina yanu. Bolungama Bazani zunguluka chifukwa mwanichitila va bwino.

Chapter 143

¹ Salimo ya Davide. mvelani pempelo yanga, Yehova; mvelani kupapata kwanga. Chifukwa cho kukulupilika kwanu na chilungamo chanu, niyankeni! ² Musangene muchiweluzo na kapolo wanu, pakuti pamenso panu palibe wolungama. ³ Mudani akonka moyo wanga; anishanyaulila pansi; Aninkazika mumudima monga bantu bamene banafa kudaladala. ⁴ Muzimu wanga wacomoka mukati mwanga; mutima wanga wavutika mukati. ⁵ Nikumbukila masiku yakudala; Niganizila ntchito zanu zonse; Nimaganizila pavamene mwakwanilisa. ⁶ Natambasula manja yanga kuli imwe; umoyo wanga umvela njota ya imwe mziko yo yuma. Selah ⁷ Niyankeni msanga, Yehova, pakuti mzimu wanga wacomoka. Musabise nkope yanu, kuti nisankale monga bantu bogwela mu chimugodi. ⁸ Nimvele pangano yanu yokulupilika kuseni. pakuti nikulupilila muli imwe. Nnilangizeni njila yakuti niyendelmo, pakuti ndikwezeka umoyo wanga kuli imwe. ⁹ Nipulumuseni kubadani banga, Yehova; Nitabila kuli imwe kubisama. ¹⁰ Nipunzseni kuchita chifunilo chanu, pakuti imwe ndimwe Mulungu wanga. Mzimu wanu wabwino unisogolele mziko yachilungamo. ¹¹ Yehova, chifukwa cha zina yanu, munisunge na moyo; mu chilungamo chanu muchose umoyo wanga mumavuto. ¹² Muchipangano chanu chosani badani banga ndipo muwononge badani bonse ba umoyo wanga, pakuti ine ndine mtumiki wanu.

Chapter 144

¹ Salimo ya Davide. Wolemekezeka Yehova, tantwe yanga, wopunzisa manja yanga kunkondo, na vimbombo vanga kunkondo. ² Imwe ndimwe pangano yanga yokulupilika na chipupa changa, nsanja yanga itali, na wonipulumusa, chishango changa, na wamene nimatamangilako, wamene anagonjesa bamitundu pansi panga. ³ Yehova, muntu nindani kuti mumusamalile, kapena mwana wa muntu nindani kuti mumukumbukile? ⁴ Muntu ali monga mpepo; masiku yake yali monga chimfwile chopita. ⁵ Mbilisani kumbi, nakuyi selusa, Yehova; Gwilani mapili nakuyachosa chusi. ⁶ Tumani tuleza naku mwazya badani banga; ponya mivi yako, nakubabweza mumusokonezo. ⁷ Tambululani kwanja yanu kuchokela kumwamba; nipulumuseni mumanzi yambili, mumanja ya balendo. ⁸ Pakamwa pao pakamba boza, ndipo kwanja yao yamanja niyaboza. ⁹ Nizakuimbilani nyimbo yasopano, MULUNGU; Nizayimba voyimbila va zingwe khumi, Imwe bamene mupulumusa mafumu, ¹⁰ bamene munapulumusa Davide mtumiki wanu ku lupanga yoyipa. ¹¹ Nipulumuseni na kunipoka mukwanja mwa balendo. Pakamwa pabo pakamba boza, ndipo kwanja yao yamanja niyaboza. ¹² Bana batu bamuna bankale monga vomela vamene vakula msinku mu ufana wao, na bana batu bakazi monga mizati yapa kona yobezewa, yo oneka monga nyumba zaufumu. ¹³ Vimpaka watu vinkale na vipaso va mitundu iliyonse, ndipo nkosa zatu zibale masausande nama sausande mu minda zatu. ¹⁴ Pamenepo ng'ombe zatu zizabala bana bambili. Palibe amene azaboola vipupa watu; sipazankala kupoka, kapena kulila munjila zatu. ¹⁵ nibodalisika bantu bamene bali namadaliso yamene aya; nibodalisika bantu bamene Mulungu wawo ni Yehova.

Chapter 145

¹ Salimo ya matamando. ya Davide. Nizakutamandani, imwe Mulungu wanga, Mfumu; nizalemekeza zina yanu ntau zonse. ² Nizakudalisani masiku onse; Nizalemekeza zina yanu mpaka muyayaya. ³ Yehova ni mukulu, ayenela kulemekezewa kukulu; Ukulu wake siwochita kusakila. ⁴ Mubadwo winango uzalemekeza vochita vanu ku mubadwo winango, ndipo uzazibisa vampamvu zanu. ⁵ Nizaganizila ukulu wa ulemelelo wanu, na vochita vanu vabwino. ⁶ Beve bazakamba pa mpamvu za nchito zanu zabwino, ndipo nizakamba ukulu wanu. ⁷ Bazakamba va kuwama kwa mtima wanu, ndipo bazaimba va chilungamo chanu. ⁸ Yehova ndiye wachisomo, ni wachifundo, wosakwiya msanga, ni wa chifundo chikulu. ⁹ Yehova ni wabwino kuli bonse; chifundo chake chili pa nchito zake zonse. ¹⁰ vonse vamene munapanga vizakuyamikilani, Yehova; ¹¹ Beve bazakamba pa ulemelelo wa ufumu wanu, ndipo bazakamba pa mpamvu zanu. ¹² Bazazibisa muntu alionse pa zinchito za mpamvu za Mulungu na kuwama kwa ulemelelo wa ufumu wake. ¹³ Ufumu wanu ndiye ufumu wosasila, na ulamulilo wanu unkalilila mumibadwo yonse. ¹⁴ Yehova atandizila bonse bamene bakugwa na kuyimilika bonse bobelama. ¹⁵ Menso yabo bonse yayembekeza imwe; mumabapasa chakudya chao pa ntau yoyenela. ¹⁶ Mumasegula kwanja yanu naku kutilisa chilakolako cha volengewa vonse. ¹⁷ Yehova ni wolungama mujila zake zonse, ni wokulupilika muvochita vake vonse. ¹⁸ Yehova ali pafupi na bonse bamene baitana kuli eve, kuli bonse bamene baitana pali eve mokukulupilika. ¹⁹ Amakwanilisa vofuna va bamene bamamulemekeza; amamvela kulila kwao na kuba pulumusa. ²⁰ Yehova amayangani onse bamene bamukonda, koma azawononga boipa bonse. ²¹ Pakamwa panga pazakamba matamando ya Yehova; nena matamando a Yehova; muntu wonse adalise zina yake yoyela muyayaya.

Chapter 146

¹ Tamandani Yehova. Lemekeza Yehova, moyo wanga. ² Ndidzalemekeza Yehova ndi moyo wanga wonse; Ndidzayimbira zolemekeza Mulungu wanga pokhala ndilipo. ³ Musakhulupirire akalonga, kapena anthu, amene mulibe chipulumutso mwa iwo; ⁴ Mpweya wa moyo wa munthu ukatha, amabwerera kunthaka; tsiku limenelo zolingalira zake zatha. ⁵ Wodala iye amene ali ndi Mulungu wa Yakobo kuti akhale mthandizi wake, amene chiyembekezo chake chili mwa Yehova Mulungu wake. ⁶ Yehova analenga kumwamba ndi dziko lapansi, nyanja, ndi zonse ziri m'mwemo; asunga kukhulupirika kosatha. ⁷ Iye amachitira chilungamo otsenderezedwa, ndipo amapereka chakudya kwa anjala. Yehova amamasula omangidwa; ⁸ Yehova atsegula maso akhungu; Yehova amautsa owerama; Yehova amakonda anthu olungama. ⁹ Yehova asunga alendo m'dziko; akwezera ana amasiye ndi akazi amasiye, koma atsutsana ndi oipa. ¹⁰ Yehova adzalamulira kosatha, Mulungu wako, Ziyoni, ku mibadwomibadwo. Tamandani Yehova.

Chapter 147

¹ Tamandani Yehova, pakuti kuyimbira zolemekeza Mulungu wathu n'kwabwino; nzokondweretsa, ndipo kuyamika koyenera. ² Yehova amanganso Yerusalemu; asonkhanitsa anthu obalalika a Israyeli. ³ Achiritsa osweka mtima, namanga mabala awo; ⁴ Amawerenga nyenyezi; azitchula mayina onsewo. ⁵ Mbuye wathu ndi wamkulu, Ngwamphamvu zake; kuzindikira kwake sikungayesedwe. ⁶ Yehova akwezera opsinjika; Agwetsera pansi oipa. ⁷ Imbirani Yehova ndi chiyamiko; imbirani Mulungu wathu zolemekeza ndi zeze. ⁸ Amaphimba thambo ndi mitambo, nakonzera dziko mvula, nameretsa msipu pamapiri. ⁹ Amapereka chakudya kwa nyama ndi ana akhungubwe pamene akulira. ¹⁰ Sakondwera ndi mphamvu ya kavalo; sakondwera ndi miyendo yamphamvu ya munthu; ¹¹ Yehova akondwera ndi iwo akumlemekeza, amene ayembekezera kukhulupirika kwa pangano lake. ¹² Lemekeza Yehova, Yerusalemu; tamanda Mulungu wako, Ziyoni. ¹³ Pakuti alimbitsa mipiringidzo ya zipata zako; adalitsa ana anu pakati panu.

¹⁴ Amabweretsa mtendere m'malire anu; amakukhutitsani ndi tirigu wokometsetsa. ¹⁷ Apereka matalala ngati zinyenyewazi; ndani angathe kupirira kuzizira kumene atumiza? ¹⁸ Atumiza lamulo lake, nazisungunula; apangitsa mphepo kuwomba, ndi madzi ayenda. ¹⁹ Iye analengeza mawu ake kwa Yakobo, malemba ake ndi maweruzo ake olungama kwa Isiraeli. ²⁰ Iye sanachite zimenezi ndi mtundu wina uliwonse, ndipo malamulo ake sakuwadziwa. Tamandani Yehova.

Chapter 148

¹ Yamikani Yehova. Lemekezani Yehova, imwe muli kumwamba; mu yamikani, imwe muli kumwamba. ² Mulemekezeni, angeli bake bonse; mulemekezeni, makamu bake bonse. ³ Mulemekezeni, zuba na mwezi; mulemekezeni, imwe nyeyezi zobeka. ⁴ Mulemekezeni, m'mwamba mwamba, ndi inu madzi akumwamba; ⁵ Alemekeze dzina la Yehova, pakuti iye analamulira, ndipo zinalengedwa. ⁶ ndipo anazikhazikitsa ku nthawi za nthawi; adapereka lamulo lomwe silidzasintha. ⁷ Mlemekezeni ku dziko lapansi, zinsomba inu, ndi zozama zonse za m'nyanja, ⁸ moto ndi matalala, matalala ndi mitambo, mphepo yamkuntho yakukwaniritsa mawu ake. ⁹ Mtamandeni, inu mapiri, ndi zitunda zonse, mitengo yazipatso, ndi mikungudza yonse, ¹⁰ nyama zakuthengo ndi zoweta zonse, zokwawa, ndi mbalame za mapiko. ¹¹ Lemekezani Yehova, inu mafumu a dziko lapansi, ndi mitundu yonse, akalonga ndi onse olamulira padziko lapansi, ¹² anyamata ndi atsikana, okalamba ndi ana. ¹³ Onse alemekeze dzina la Yehova, pakuti dzina lake lokha lakwezeka, ndipo ulemerero wake wafikira dziko lapansi ndi kumwamba. ¹⁴ Iye wakweza nyanga ya anthu ake kuti atamandidwe kuchokera kwa okhulupirika ake onse, ana a Isiraeli, anthu amene ali pafupi naye. Tamandani Yehova.

Chapter 149

¹ Yamikani Yehova! Imbilani Yehova nyimbo yasopano; imbani matamando yake m'msonkhano wa okhulupilika.
² Israyeli akondwele muli wamene anabapanga; bantu ba ku Ziyoni bakondwele muli mfumu yao. ³ Alemekeze zina yake na kuvina; amuimbile zolemekeza na lingaka na zeze. ⁴ Pakuti Yehova akondwela na bantu bake; amalemekeza ozichepesa na chipulumuso. ⁵ Okhulupilika ba kondwele na ulemu wamene uyu; ayimbe mokondwela pakama pao. ⁶ Mayamiko ya Mulungu yankhale mukamwa mwao na lupanga yakutwa konsekonse mu kwanja mwao, ⁷ kubwezela cilango ku mitundu na kulanga bantu. ⁸ Bazamanga ma mfumu yao na maunyolo na bolemekezeka bao bazamanga maunyolo ya nsimbi. ⁹ Bazachita chiweluzo cholembewa. Ichi chiza nkala ulemu kuli batumiki bake bonse bokhulupilika. Yamikani Yehova.

Chapter 150

¹ Tamandani Yehova! Lemekezani Yehova m'malo yake yoyela; mulemekezeni m'mwamba wamphamvu. ² Mulemekezeni chifukwa cha ntchio yake yamphamvu; Mulemekezeni chifukwa cha ukulu wake opambana. ³ Mulemekezeni na kulila kwa lipenga; mutamandeni na zeze ndi zeze. ⁴ Mulemekezeni na malingaka na kuvina; mutamandeni na voyimbila va vingwe na zoimbila. ⁵ Mulemekezeni na vinganga vomveka; mutamandeni na vinganga vomveka bwino. ⁶ Lekani vilichonse vamene vili na umoyo vitamande Yehova. Tamandani Yehova.

Chapter 20

¹ Kwa woyimba wamkulu. Salmo la Davide. Lekani Yehova akutanizeni pa siku ya mavuto; lekani zina ya Mulungu wa Yakobo ikuchingilileni ² nakutuma tandizo kuchokela ku malo yoyela kukutandizani imwe kuchoka ku Ziyoni. ³ Lekani akumbukile vonse vopasa vanu na kuvomela nsembe zoshoka zanu. Sela ⁴ Lekani akupase zamene mutima wako ufuna na kukwanilisa zamene uganizilapo. ⁵ Ndipo tizakondwela pa kupambana kwanu, muzina ya Mulungu wathu, tizanyamula ndembela. Lekani Yehova akupaseni zopempa zanu zonse. ⁶ Manje niziba kuti Yehova azapulumusana bozozedwa bake; azamuyanka kuchokela kumwamba kwake koyela ndi mphamvu ya kwanja kwake kwamanja kwamene kumapulumusana. ⁷ Benangu bakulupilila mu magaleta na benangu mu makavalo, koma ife tikulupilila mu zina ya Yehova Mulungu wathu. ⁸ Bazabwelesewa pansu na kugwa, koma ife tizanyamuka na kuimilila! ⁹ Yehova, pulumusani mfumu; titandizeni tikayitana.

Chapter 21

¹ Kwa woyimba wamkulu. Salmo la Davide. Mfumu ikondwela mu mpamvu zanu, Yehova! Iye amasangalala kwambili na chipulumuso chamene mumapeleka! ² Mwamupasa zofuna mutima wake ndipo simunagwililile kumbuyo kupempa kwa milomo yake. Selah ³ Chifukwa mumamubwelesela madaliso yolemela; munaika pamutu pake kolona wa golide yoyengeka. ⁴ Anakupempani umoyo; munamupasa; munamupasa utali wa masiku yake ku kwamuyayaya. ⁵ Ulemelelo wake ni ukulu chifukwa cha kupambana kwanu; mwamuvalika ulemelelo na ukulu. ⁶ Chifukwa mumupasa madaliso yosata; mumamukondwelesa nachikondwelelo cha kunkalapo kwanu. na kukondwela pamenso panu. ⁷ Chifukwa mfumu akulupilila muli Yehova; kupitila mu chipangano chokulupilika cha wakumwamba mwamba sazagwendezeka. ⁸ Kwanja kwanu kuzagwila bonse badani banu; kwanja kwanu kwa manja kuzagwila bamene bakuzonda iwe. ⁹ Pa ntawi ya ukali wanu, muzabashoka monga munganjo yamulilo. Yehova azabashoka muukali wake, na mulilo uzabanyekesa. ¹⁰ Uzawononga mbewu yawo paziko yapansi na wobadwa kuchokela ku mutundu wa bantu. ¹¹ Chifukwa banapingila voipa mosushana na iwe; banabala maganizo yamene sibazakwanisa! ¹² Chifukwa muzababweza kumbuyo; uzabapangila uta wako pasogolo pawo. ¹³ Mukwezedwe, Yehova, mu mpavu zanu; tizaimba na kutamanda mpavu zanu.

Chapter 22

Kwa woyimba wamukulu; nkazikisani "Mayimbidwe ya gwape." Salmo ya Davide. ¹ Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwanikanila chani? Nichifukwa chani muli kutali kunipulumusa na kutali na mau yakubaba kwanga? ² Mulungu wanga, nimalila muntawi ya muzuba, koma simumayanka, na usiku sininkala zii! ³ Koma ndimwe woyela; mumankala monga mfumu na matamando ya Israyeli. ⁴ Makolo yatu yanakukulupililani imwe; yanakulupilila Imwe, ndipo munabapulumusa. ⁵ Banalilila kuli imwe ndipo banapulumusiwa. Banakulupilila muli imwe ndipo sibanakumudwe. ⁶ Koma ine ndine nyongolosi osati munthu, chonyozewa ku muntu ndipo osuliwa kuli banthu. ⁷ Bonse bamene baniona banitonzya; baniseka, bamapukunya mitu yawo pali ine. ⁸ Bakamba kuti, "Akulupilila muli Yehova; lekani Yehova amupulumuse. Lekani amupulumuse, chifukwa asangalalila muli eve." ⁹ Chifukwa munanichosa ine mumimba; munalengesa ine kukulupilila muli imwe pamene ninali kuma ziba yaba mai. ¹⁰ Ninaponyewa kuli imwe kuchokela mumimba; ndimwe Mulungu wanga kuchokela pamene ninali mumimba muli ba mai! ¹¹ Musankale kutali na Ine, chifukwa mavuto yali pafupi; kulibe ngankale umozi onitandiza. ¹² Ng'ombe zambili zanizunguluka; ng'ombe zampamvu zaku Basana zanizunguluka. ¹³ Zisegula makamwa mosushana naine mongankalamu yobangula pamene ing'amba nyama yake. ¹⁴ Ndine otiliwa monga manzi, na mafupa yanga yali yopindamuka. Mtima wanga uli ngati sera; umasungunuka mukati mwanga. ¹⁵ Mpamvu zanga zayuma ngati mbiya; lulime lwanga lumamamatila pakamwa panga. Mwaniika mudoti ya imfa. ¹⁶ Chifukwa bagalu banizunguluka; gulu ya ochita voipa banizinguluka; balasa manja yanga na mendo yanga. ¹⁷ Ningabelenge mabonzo yanga. Yaona na kungana ine. ¹⁸ Bagabana vovala vanga beka beka, bachita mayele pa zovala zanga. ¹⁹ musankale kutali, Yehova; napapata yendesani kunitandiza, mpavu zanga! ²⁰ Pulumusani moyo wanga ku lupanga, moyo wanga kuchoka ku zikadabo za bagalu. ²¹ Ndipulumuseni kuchoka mukamwa mwa mukango; nipulumuseni kuchoka ku minyanga za ng'ombe zamusanga. ²² Nizalalikila zina yanu kuli ba bale banga; pakati pa musonkano nizakutamandani imwe. ²³ Imwe bamene muyopa Yehova, mutamandeni! Imwe bonse bana ba Yakobo, mulemekezeni! Imililani mu mukuyopa eve, bonse imwe bana ba Isiraeli. ²⁴ Chifukwa sanaonelemo kapena kunyansidwa na kusauka kwa ovutika uyo; Yehova sanabise nkope yake kuli eve; pamene wovutika analila kuli eve, ananvela. ²⁵ Kuyamika kwanga kuzankala chifukwa cha iwe mu musonkano ukulu; nizakwanilisa zamene ninalonjeza pamenso pa bamene bayopa Yehova. ²⁶ Odyakiliwa bazadya na kukuta; bamene basakila Yehova bazamulemekeza. Lekani mitima yanu inkale muyayaya. ²⁷ Bonse bantu ba paziko lapansi bazakumbukila na kutembenukila kuli Yehova; yonse mabanja ya maziko yazagwada pamenso panu. ²⁸ Chifukwa ufumu niwa Yehova; ndiye wolamulima wa maziko. ²⁹ Wolemela bonse bapa ziko lapansi bazadya na kulambila; bonse bamene baselukila kuyenda kudoti bazagwada pamenso panga, bamene sibangasunge moyo wawo. ³⁰ Mubadwe wamene ubwela uzamutumikila; bazauza mubadwe obwela wa Yehova. ³¹ Bazabwela na kubauza pazakukulupilika kwake; bazakamba kubantu bamene bakalibe kubadwa vamene anachita.

Chapter 23

¹ Salmo la Davide. Yehova ndiye mbusa wanga; sinizasoba kantu. ² Amanigonesa mumusipu wobilibila; anisogolela kumanzi yabata. ³ Amabweza umoyo wanga; Amanisogolela munjila chifukwa cha zina yake. ⁴ Ngankale niyenda muchigwa cha mumudima, sinizayopa zopweteka, chifukwa muli na ine; ndodo yanu na vogwilisa ncito vanu vimanitontoza. ⁵ Mumanikonzela tebo pamenso pa badani banga; mwazozza mutu wanga na mafuta; chiko changa chisefukila. ⁶ Zoona zabwino na chipangano chokulupilika vizanikonka mumasiku ya umoyo wanga wonse; ndipo nizankala mu nyumba ya Yehova mu masiku ya umoyo wanga bonse!

Chapter 24

¹ Salmo la Davide. Ziko lapansi ni ya Yehova, na zozulamo zonse, ziko lapansi, na bonse bamene bankalamo. ² Chifukwa anaimbisa pa nyanja na kuinkazikisa pa mimana. ³ Nindani azakwela pili ya Yehova? Nindani azaimilila mu malo yake yoyela? ⁴ Wamene ali na manja yoyela na mutima woyera; wamene sanakweke za boza, ndipo sanalumbilile kuti achite zonyenga. ⁵ Azalandila madaliso kwa Yehova na chilungamo kuchoka kuli Mulungu wa chipulumuso. ⁶ Ndiye mubadwe wa bamene bamufuna eve, bamene basakila nkope ya Mulungu wa Yakobo. Selah ⁷ Kwezani mitu yanu, mageti imwe; Kwezekani, imwe viseko vosasila, kuti Mfumu ya ulemelelo ingenemo! ⁸ Nanga Mfumu ya ulemelelo nindani? Yehova, wolimba ndiponso wampamvu; Yehova, wampamvu munkondo. ⁹ Kwezani mitu yanu, mageti imwe; Kwezekani, inu viseko vosasila, kuti Mfumu ya ulemelelo ingenemo! ¹⁰ Nanga Mfumu ya ulemelelo nindani? Yehova wa makamu, ndiye Mfumu ya ulemelelo. Selah

Chapter 25

¹ Salmo la Davide. Kuli imwe, Yehova, nikweza moyo wanga; ² Mulungu wanga, nikulupilila imwe; Musalengese kuti ine ninyozewe; musalengese badani banga kusangalala mopambana pali ine. ³ Musaleke wamene ayembekezela pali imwe achitiwe manyazi; lekani bamene bachita zachinyengo kulimbe mulandu bachitiwe wakuyembekezera Inu; achite manyazi iwo akuchita zachiwembu popanda chifukwa! ⁴ Munizibise ine njila zanu, Yehova; nipunziseni njila zanu. ⁵ Nisogoleleni mu chazoona chanu na kunipunzisa; chifukwa ndimwe Mulungu wa chipulumuso changa; niyembekezela pali imwe siku yonse. ⁶ Kumbukilani, Yehova, machitidwe yanu ya chifundo na chipangano cha kukulupilika kwanu; chifukwa vilipo kuchokela kale. ⁷ Musaganizile pa machimo yaku ufana wanga kapena kusanvelela kwanga; munikumbukile na chipangano chanu chokulupilika chifukwa cha ubwino wanu, Yehova! ⁸ Yehova ni wabwino ndiponso wolungama; chifukwa chake amapunzisa ochimwa njila. ⁹ Amasogolela ozichepesa mu vinthu vili bwino na kubapunzisa njila yake. ¹⁰ Njila zonse za Yehova niza chifundo na kukulupilika kwa beve basunga chipangano chake na malamulo yake. ¹¹ Chifukwa cha zina yanu, Yehova, munikululukile zolakwa zanga, chifukwa ni chachikulu. ¹² Nindani muntu wamene amayopa Yehova? Yehova azamulangiza njila yamene afunika kusanka. ¹³ Umoyo wake uzayendela pamozi na zabwino; na wobadwa bake bazalandila ziko. ¹⁴ Ubwenzi wa Yehova ni wa bantu bamene bamamulemekeza, ndipo amabalengesa kuziba chipangano chake kuli beve. ¹⁵ Menso yanga yali pali Yehova ntawi zonse; chifukwa azachosa mendo yanga kuchoka ku sumbo. ¹⁶ Pindamukilani kuli ine na kuninvelela chifundo; chifukwa nili neka ndiponso wozunzika. ¹⁷ Mavuto ya mutima wanga yakula; nichoseni kuchoka mumasauso yanga! ¹⁸ Onani kuvutika kwanga na nonilemesa; nikululukileni machimo yanga yonse. ¹⁹ Onani badani banga, ndipo bali bambili; banizonda na kuzonda kwachongo. ²⁰ Chingilizani moyo wanga na kunipulumusa ine; musalengese ine banichepese, chifukwa nimatabila kuli imwe! ²¹ Lekani Ungwilo na kuimilila vinisunge ine, chifukwa niyembekezela muli imwe. ²² Pulumusani Israyeli, Yehova, kuchoka ku yonse mavuto yake!

Chapter 26

Salmo la Davide. ¹ Niweluzeni, Yehova, chifukwa nayenda na ungwilo; Nakulupilila Yehova mosagwendezeka. ² Nioneni, Yehova, nakuniyesa; yesani kuyela kwa mukati mwanga na mumutima mwanga! ³ Chifukwa chipangano chanu chokulupilika chili pamenso panga, ndipo nimayenda muchilungamo chanu. ⁴ Sinicheza na bantu bachinyengo, kapena kupezeka na bantu balibe chilungamo. ⁵ Nimazonda musankano wa wochita voipa, ndipo sinimankala na woipa. ⁶ Nimasamba mumanja mwanga mukusalakwa, na kuzunguluka guwa yanu yansembe, Yehova, ⁷ kuyimba nyimbo yonveka ya kutamanda na kukamba zonse nchito zanu zabwino ⁸ Yehova, nikonda nyumba yamene munkalamo, kumalo kwamene ulemelelo wanu unkala. ⁹ Musanipyangile pamozi na wochimwa, kapena umoyo wanga na bantu okesa mwazi, ¹⁰ bamene mumanja mwawo muli chibembu, na kwanja kwawo kwamanja kozula na kubosha. ¹¹ Koma monga ine, nizayenda mu ungwilo; niomboleni na kunichitila chifundo. ¹² Mwendo wanga umaimilila pantaka; mumisonkano nizadalisa Yehova!

Chapter 27

¹ Salmo la Davide. Yehova ni nyali yanga na chipulumuso changa; Nindani wamene ningayope? Yehova ni kotabila kwa moyo wanga; nindani wamene ningayope? ² Pamene wochita voipa banabwela kuli ine kuti badye tupi yanga, bachongo na badani banga banazibuntula na kugwa. ³ Ngankale gulu ya bankondo yanizungulila, mutima wanga siuzayopa; ngankale nkondo yanyamuka mosusana na ine, ngankale pamene apo nizankala olimba. ⁴ Chintu chimozi namufunsa Yehova, ndipo nizachifuna: kuti ninkale munyumba ya Yehova yonse masiku ya umoyo wanga, kuti nione kuoneka bwino kwa Yehova na kuganizilapo mu tempele yake. ⁵ Chifukwa pa siku yamavuto azanibisa mu malo yake; mu chovininkila chake mu tenti azanibisa. Azaninyamula pamwamba pa mwala! ⁶ Ndipo mutu wanga uzakwezedwa pamwamba kuchila badani banga wonizungulila, ndipo nizapeleka nsembe zachikondwelelo mu chihema! Nizaimba na kuimba nyimbo kwa Yehova! ⁷ Nvelani, Yehova, mau yanga pamene nilila! Nichitileni chifundo, na kuniyanka! ⁸ Mutima wanga ukamba pali imwe, "Funa nkope yake!" Nima funa nkope yanu, Yehova! ⁹ Musabise nkope yanu kuli ine; musamutailile mutumiki wanu muukali! mwankala mutandizi wanga; musanisiye kapena kunikana, Mulungu wa chipulumuso changa. ¹⁰ Ngakale batate na bamayi banga banikane, Yehova azanilandila. ¹¹ Nipunziseni njila yanu, Yehova! Munisogolele panjila yolunjika chifukwa cha badani banga. ¹² Musanipeleke ku zofuna za badani banga, chifukwa mboni zaboza zanyamuka mosushana naine, ndipo bapema chongo! ¹³ Nganichani chinanichitika kuli ine ngati sininakulupilile kuti nizaona ubwino wa Yehova mu ziko ya bantu bamoyo? ¹⁴ Yembekezela pali Yehova; nkala olimba, ndipo leka mutima wako unkale olimba! Yembekeza pali Yehova!

Chapter 28

¹ Salmo la Davide. Kuli imwe, Yehova, Nalilila; mwala wanga, Musanisule. Ngati simuzaniyanka ine, nizakonka awo bamene banayenda pansi kumanda. ² Nvelani mau ya kupempa kwanga pamene niitana kufuna tandizo kuli imwe, pamene nanyamula manja yanga kumalo yanu yoyela! ³ Musanifendezele pamozi na woipa, bamene bachita voipa, bamene bakamba mutendele na bali pafupi nawo koma bali navoipa mumitima yawo. ⁴ Bapaseni vamene viyenela nchito zawo na kubabwezela vamene voipa vao vifuna; babwezeleni pazincito zawo za manja kubapasa zamene zibafunikila. ⁵ Chifukwa zibaziba zinchito za Yehova kapena nchito za manja yake, azabapasula ndipo sazabamanga futi. ⁶ Wodalisika ankale Yehova chifukwa anvela mau ya kupapata kwanga! ⁷ Yehova ni mpamvu zanga na chikopa changa; mutima wanga ukhulupilila muli eve, ndipo natandiziwa. Chifukwa chake mutima wanga ukukondwela kwambili, ndipo nizamulemekeza mu kuyimba. ⁸ Yehova ni mpamvu ya banthu bake, ndipo ndiye motabila mopulumukila wozozedwa bake. ⁹ Pulumusani bantu banu na kudalisa cholowa chanu. Munkale mubusa wawo na kubanyamula kwamuyayaya.

Chapter 29

¹ Salmo la Davide. Pasani kwa Yehova, imwe bana ba Mulungu, pelekani kwa Yehova ulemelelo na mphamvu. ² Pelekani kwa Yehova ulemelelo woyenelela zina yake. Gwadani kwa Yehova mu ulemelelo wa chiyelo! ³ Mau a Yehova yamveka pamwamba pa manzi; Mulungu wa ulemelelo yagunda, Yehova agunda pa manzi yambili. ⁴ Mau ya Yehova ni yampamvu; mau ya Yehova ni yaulemelelo. ⁵ Mau ya Yehova yatyola mikunguza; Yehova atyolatyola mikunguza yaku Lebanoni. ⁶ Amapanga Lebano ngati mwana wa ng'ombe, na Sirioni ngati mwana wa ng'ombe. ⁷ Mau ya Yehova yamatuma vimbilimbili va mulilo. ⁸ Mau ya Yehova agwedeza chipululu; Yehova yagwendeza chipululu; Yehova agwendeza chipululu cha ku Kadesi. ⁹ Mau ya Yehova yalengesa mutengo ya thundu kupindamuka na kuswa nkalango. Aliyense mu tempele yake akuti, "Ulemerero!" ¹⁰ Yehova amankala monga mfumu pamwamba pa chigumula; Yehova amankala monga mfumu muyayaya. ¹¹ Yehova amapasa mpavu kubantu bake; Yehovah amadalisa bantu bake na mutendele.

Chapter 30

¹ Nizakukwezani, Yehova, chifukwa mwanikweza ine pamwamba ndipo simunalole badani banga kusangalala chifukwa cha ine. ² Yehova Mulungu wanga, ninalilila kwa imwe kufuna tandizo, ndipo munanipolesa. ³ Yehova, mwanitulusa kumanda; mwanisunga na moyo kuti kuchoka kuyenda kumanda. ⁴ Imbani matamando kwa Yehova, inu okhulupirika ake; Yamikani pokumbukira chiyero chake. ⁵ Chifukwa ukali wake uli koma wakantawi; koma kuwama mutima kwake nikw ntawi yaumoyo onse. Kulila kumabwela usiku, koma kukondwela kumabwela kuseni. ⁶ Mukulimba mutima ninati, "Sinizagwendezeka." ⁷ Yehova, mwa kuwama mutima kwanu munaninkazikisa monga lupili lolimba; koma pamene munabisa nkope yanu, ninavutika. ⁸ Ninalilila kwa imwe, Yehova, ndipo ninafuna kuwama mutima kuchoka kuli Ambuye wanga. ⁹ Ni umushe bwanji uli mu magazi yanga, ngati nayenda pansi mumanda? Kodi doti izakuyamikani? Kodi izakamba pa kukulupilika kwanu? ¹⁰ Nvelani, Yehova, ndipo nkalani nachifundo pali ine! Yehova, nkalani tandizo yanga. ¹¹ Mwasandusa kulila kwanga kunkala kuvina; mwachosapo chisaka pali ine na kunivalika chimwemwe. ¹² Ndipo manje ulemelelo wanga uzakuyimbilani imwe zolemekeza sinizankala chete; Yehova Mulungu wanga, nizakuyamikani muyayaya;

Chapter 31

Kuli woyimba mukulu. Salmo ya Davide. ¹ Muli imwe, Yehova, nitabilamo; musanileke kuti ninyozedwe. Nipulumuseni muchilungamo chanu. ² Nvelani kuli ine; nipulumuseni moyendesa; nkalani mwala wanga wotabilamo, linga ya kunipulumusa. ³ Pakuti ndiwe mwala wanga na malo yachitetezo yanga; mwaicho chifukwa cha zina yanu, munisogolele na kunilangiza. ⁴ Munichose muli choteyesa chamene banibisila, pakuti ndimwe chotabila changa. ⁵ Mumanja yanu naika muzimu wanga; muzaniwombola, Yehova, Mulungu wokulupilika. ⁶ Nizonda bantu botumikila mafano yachabe, koma nikulupilila muli Yehova. ⁷ Nizakondwela naku sangalala muchipangano chanu chokulupilika, chifukwa munawona kusauka kwanga; muziba kusinjiwa kwa moyo wanga. ⁸ Simunanipeleke mumanja ya badani banga. Mwaimika mendo yanga mumalo yakulu yoseguka. ⁹ Nichitileni chifundo, Yehova, chifukwa ndili mumasauso; maso yanga yalema na chisoni na moyo wanga na tupi yanga. ¹⁰ Pakuti moyo wanga walema na chisoni, na zaka zanga na kubuula. Mphamvu zanga zatha chifukwa cha machimo yanga, ndipo mafupa yanga yalefuka. ¹¹ Chifukwa cha badani banga bonse, bantu banipepusa; bonkala pafupi panga badabwa na makalidwe yanga, ndipo boniziwa balina namanta. Bamene baniona munjila bamanitaba. ¹² Naibaliwa monga muntu wokufa wamene alibe omuganizila. Ndili ngati mphika wosweka. ¹³ Pakuti namva kubelebesha kwa bambili, nkani zoyofya zochokela kumbali zonse pamene banikonzela chiwembu. Bamakonzela chiwembu chotenga umoyo wanga. ¹⁴ Koma nikulupilila muli imwe, Yehova; nakamba kuti, "Imwe nimwe Mulungu wanga." ¹⁵ Ntawi yanga ili mumazanja yanu. Nipulumuseni chokela mumanja ya badani banga na kuli bamene bakunitamangisa. ¹⁶ Muwalise nkope yanu pali kapolo wanu; nipulumuseni muchipangano chanu chokulupilika. ¹⁷ Musanilekele kuti ninyozedwe, Yehova; chifukwa niyitanakuli imwe! boipa anyozewe! Lekani bankale chete kumanda. ¹⁸ Milomo yaboza inkale chete yamene ikamba pali bolungama motukwana na mwano. ¹⁹ Ni ubwino wanu waukulu wamene mwaunjikila bamene bakuyopani, kuti muchitile abo bamene batabila kuli imwe pamaso pa bana ba bantu bonse! ²⁰ Mumalo yobisalamo pamaso panu, mubisa ku chiwembu cha bantu. Mubabisa pobisalila chiwawa cha malilime. ²¹ Alemekwezeka Yehova, pakuti ananionesa chipangano chake chodabwisa pamene ninali mumuzi wozingidwa; ²² Ngakale nikamba kuti mukufulumila kwanga, "Nachosewa pamaso panu, "koma munamva pempho yanga yofunila pamene ninalila kuli imwe. ²³ Kondani Yehova, imwe bonse okulupilika. Yehova amateteza bokulupilika, koma amabwezela mokwanila ozikuza. ²⁴ Limbani mutima, bonse bamene mukulupilila Yehova.

Chapter 32

Salmo ya Davide. A machili. ¹ Wodala muntu wamene akululukidwa zolakwa zake, wamene machimo yake yavimbiwa. ² Wodala muntu wamene Yehova samuwelengela cholakwa, ndipo mu muzimu wake mulibe kunama. ³ Pamene ninankala chete, mafupa yanga anaphwa na kubuula siku yonse. ⁴ Pakuti muzuba na usiku kwanja yanu inali yolema pali ine. Mphamvu zanga zinafota ngati muchilime. Selah ⁵ Ndipo ninavomela choipa changa kuli imwe, ndipo sinibisa mphulupulu yanga. Ninakamba kuti, "nizaulula zolakwa zanga kuli Yehova," ndipo imwe munanikululukila zolakwa za zamachimo yanga. Selah ⁶ Chifukwa chake aliyense wa osatila wanu okulupilika azipemphela kuli imwe pa ntawi ya masautso yakulu. Pamene manzi yotamanga yasefuka, manzi siyazabafikila. ⁷ Imwe ndimwe mobisalila mwanga; muzaniteteza ku zovuta. Muzanizinguluka na nyimbo zachigonjeso. Selah ⁸ Nizakulangiza na kumipunzisa njila yamene muzayendela. Nizakulangiza na manso yanga pali imwe. ⁹ Musankale monga kavalo kapena nyuru, zamene zilibe nzeru; koma ni zingwe zobalamulila kuti bapite kwamene iwe ukufuna. ¹⁰ Woipa alina zobaba zambili, koma chipangano cha Yehova chokulupilika chizazunguluka wamene aza kulupilila muli eve. ¹¹ Sekelani muli Yehova, ndipo kondwelani, olungama imwe; pundani mokondwela, imwe bonse wongoka mutima.

Chapter 33

¹ kondwelani muli Yehova, olungama imwe; Kuyamika koyenela kuli wongoka. ² Yamikani Yehova na zeze; muimbileni nyimbo zomutamanda na zingwe ilina za zingwe zili kumi. ³ Muyimbileni nyimbo yamanje; sewelani mwaluso na kuyimba mokondwela. ⁴ Pakuti mawu a Yehova ni yolungama, ndipo zonse zamene amachita ni zolungama. ⁵ Eve amakonda chilungamo na chilungamo. Ziko yapansi lazula na kukulupilika kwa chipangano cha Yehova. ⁶ Mu mawu ya Yehova mwamba inalengewa, ndipo nyenyezi zonse zinalengewa na mpweya ya mukamwa mwake. ⁷ Asonkanisa manzi ya munyanja monga mulu; amaika nyanja muli chosungilamo. ⁸ Lekani ziko yonse yapansi iyope Yehova; lekani bonse bokala muziko yapansi amuyope. ⁹ Chifukwa anakamba, ndipo zinachitika; analamulila, ndipo chinayima pamenepo. ¹⁰ Yehova asokoneza mapangano cha mitundu; atesa zolingalila za mitundu ya bantu. ¹¹ Malingalilo ya Yehova ankala kwamuyayayaya, zolingalila za mutima wake ku mibadwomibadwo. ¹² Wodalika ni mutundu wamene Mulungu wawo ni Yehova, bantu bamene anawasanka kukala cholowa chake. ¹³ Yehova ayangana chokela kumwamba; amaona bantu bonse. ¹⁴ Chokela ku malo kwamene ankala, amayangana pansi pa bantu bonse bokala paziko yapansi. ¹⁵ Iye wamene amaumba mitima yabo bonse bamayangana zochita zawo zonse. ¹⁶ Palibe mfumu yamene ipulumusiwa na nkamu ikulu yankondo; wankondo sapulumusiwa na mpamvu zambili. ¹⁷ Kavalu ni chiyembekezo chaboza cha chigonjeso; Ngakhale wa mphanvu zambili, sangapulumusa. ¹⁸ Ona, liso ya Yehova ili pali bamene bamuyopa, pali bamene bakuyembekeza pa chipangano chake chokulupilika ¹⁹ kupulumusa umoyo yawo ku imfa nu kunkala na moyo mu ntawi ya njala. ²⁰ Tiyeembekeza Yehova; ndiye tandizo yatu na chishango chatu. ²¹ Mitima yatu imakondwela muli eve, chifukwa tikulupilila muzina yake yoyela. ²² Lekani chipangano chanu chokulupilika, Yehova, chinkale na naise pamene tiyembekezela imwe.

Chapter 34

Salmo ya Davide, pamene anazipanga kunkala wofunta pamaso ya Abimeleki, wamene anamungisa.¹ Nizatamanda Yehova ntawi zonse, matamando yake yazakala mukamwa mwanga ntawi zonse.² Nizatamanda Yehova! Opondelezewa anvele na kusangalala.³ Lemekezani Yehova pamozi na ine, tikweze zina yake pamozi.⁴ Ninafunafuna Yehova ndipo ananiyanka, ndipo ananigonjesa pa manta yanga yonse.⁵ Bamene bayangana kuli bamawala, ndipo nkope zawo zilibe manyazi.⁶ Muntu wopondelezewa analila ndipo Yehova anamunvela ndipo anamupulumusa kuchokela mumavuto yake yonse.⁷ Mungelo wa Yehova amamanga musasa kuzunguka bantu bamene bamamuyopa na kubapulumusa.⁸ Lawani ndipo muone kuti Yehova ni wabwino. Wodasika ni muntu wamene atabila kuli yeve.⁹ Yopani Yehova, imwe bantu bake boyera. Kulibe kusowa kui abo bali bamene bamuyopa.¹⁰ Tunkalamu tung'ono ntawi zina tumasowa chakudya na njala, koma abo bamene bamafunafuna Yehova sibazasoba chilichonse chabwino.¹¹ Bwelani, bana bamuna, Nvelani kuli ine. Nizakupunzisani kuyopa Yehova.¹² Nindani muntu wamene afuna moyo nakukonda masiku yambili, kuti awone zabwino?¹³ Ndipo teteza lilime yako ku zoipa ndipo teteza milomo yako kuti isanene boza.¹⁴ Choka kuzoipa na kuchita zabwino. Funa mtendere nakuyenda pambuyo pake.¹⁵ Maso ya Yehova yali pali bolungama ndipo matu yake yali ku kulira kwawo.¹⁶ Nkope ya Yehova ili pali bochita zoipa, kuti achose chikumbukilo chawo pa ziko yapansi.¹⁷ Bolungama bamalila ndipo Yehova amanvela ndipo amabapulumusa kuchokela kumavuto yawo yonse.¹⁸ Yehova ali pafupi nabo pwanyika mutima, ndipo apulumutsa abo bali namuzimu wopwanyika.¹⁹ Mavuto ya bolungama niyambili, koma Yehova amabapulumusa kuchokela kuli yonse.²⁰ Amasunga mafupa yake yonse, kulibe imozi yamene izatyoka.²¹ Zoipa zizapaya boipa. Bamene bazonda bolungama bazaweluziwa.²² Yehova amapulumusa umoyo wa kapolo wake. Palibe aliyense wamene atabira kuli eve wamene nyozeza.

Chapter 35

Salmo ya Davide. ¹ Yehova, sebenzani pali aliyense anisusa; menyani na bamene bamenyana na ine. ² Tengani chishango chanu ching'ono na chishango chikulu; ukani nakunitandiza. ³ Sebenzesani mukondo wanu na katemo kankhondo pali bamene banitamangisa; kamba ku moyo wanga, "Ndine chipulumuso chako; ⁴ Lekani bamene basakila moyo wanga bachitiwe zamanyazi naku nyozeza. Babwezelewe mumbuyo bachitisiwe manyazi abo bamene bakonza kunichitila choipa. ⁵ Bankale mankusu pamaso pa mpepo, pamene mungelo wa Yehova abapisha. ⁶ Njila zawo zinkale zokuda na nakutelela, pamene mungelo wa Yehova abapisha. ⁷ Kulibe chifukwa banyikila zoteyela zawo; palibe chifukwa banikumbila zenje ya moyo wanga. ⁸ chiwonongeko chibagwele mozizimusa. Lekani zoteyela zamene bayika kuti bani gwile. Basiyeni bagwele mwamene, kuti bawonongewe. ⁹ Koma ine nizakondwela mwa Yehova ndipo ndidzakondwera ndi chipulumutso chake. ¹⁰ Mafupa yanga yonse azakamba kuti, "Yehova, nindani ali monga imwe, wamene amapuluma ozunzika kuchokela kuli bamene bali namphamvu na baumphawi na bosoba kuchoka kuli bamene bayesa kubabela?" ¹¹ Mboni zosalungama zimaimilila; bandinenela zaboza. ¹² Bamanibwezela choipa mumalo mwa chabwino. Ndine wachisoni. ¹³ Koma, pamene anadwala, ine ndinawala chiguduli; Ndinawasala nditaweramitsa mutu wanga pachifuwa. ¹⁴ Ninayendayenda na chisoni monga mubale wanga; Ninabelama nakulila malilo monga mayi wanga. ¹⁵ Koma pamene ninapuntwa, banakondwela nakusonkana pamozi; banasonkana kususana naine, ndipo ninadabwa nawo. Ananikazula mosalekeza. ¹⁶ Bananiseka wopanda ulemu; banishetela meno na ukali. ¹⁷ Ambuye, muzayangana kwantawi itali bwanji mpaka liti? Landisani moyo wanga ku zowononga zao, moyo wanga kwa mikango. ¹⁸ Ndipo nizakuyamikani mu musonkano ukulu; Nizakutamandani pakati pa banthu bambili. ¹⁹ Musaleke badani banga baboza kukondwela pali ine; musabaleke kuchita ziwembu zawo zoipa. ²⁰ Chifukwa sibakamba zamtendele, koma bakonza mawu yaboza pali bokala muziko bantu bonkala mumutendele. ²¹ Basegula makamwa yao maningi pali ine; banakamba kuti, Eya, Eya, menso yatu yaona." ²² Mwachiwona, Yehova, musankale chete; Ambuye, musankale kutali na ine. ²³ Galamukani kuti niushe chitetezo changa; Mulungu wanga ni mbuye wanga, tetezelani mulandu wanga. ²⁴ Nitetezeleni, Yehova Mulungu wanga, chifukwa cha chilungamo chanu; musabaleke kusakondwela pali ine. ²⁵ Basakambe mumitima yawo, "Ha, tili nazamene tinali kufuna." basakambe kuti, "Tamudya." ²⁶ Bachiteni manyazi ndipo bachite manyazi bamene basangalala na kusauka kwanga. Bamene bazikweza pali ine bavale manyazi na manyazi. ²⁷ Abo bamene bafuna chilungamo changa bapunde na kukondwela; bakamba kosaleka, Yehova alemekezeke, wamene akondwela na mtendele wa kapolo wake." ²⁸ Ndipo nizakamba za chilungamo chanu, na kukutamandani masiku yonse.

Chapter 36

Oyimba mukulu. Salimo ya Davide wa nchito wa Yehova. ¹ Muntu oipa amakamba voipa kuchokela pasi pa mtima, mulibe kuyopa Mulungu pameso mwake. ² Pakuti amazivesa bwino eka, pakuganiza kuti chimo yake siizazibika na kusakondewa. ³ Mau yake niya chimo ndipo niyonama; safuna kukhala wanzelu na kuchita vabwino. ⁴ Agona pabedi, apanga mapulani yo chimwilamo; ayenda munjila yoipa; sakana voipa. ⁵ Chipangano chachikhulupililo chako, Yehova, chifika kumwamba; kukhulupilika kwanu kufika mumakumbi. ⁶ Chilungamo chanu chili ngati malupili ya Mulungu; Viweluzo vanu vili ngati manzi yakuya. Yehova, musunga bantu na nyama. ⁷ Chipangano chachikulupililo chanu ni chamtengo ukulu manigi, Mulungu! Bantu bamatabila mumthunzi wamapako banu. ⁸ Bamadyelela pavambili va munyumba yanu; mubaleka kumwa mumsinje ondwelesa imwe. ⁹ Pakuti imwe muli kasupe wa moyo; m'kuyela kwanu tizawonamo kuyela. ¹⁰ Kulisakoni chipangano chanu chachikulupilo mofikapo kuli bamene bakuzibani, kuteteza mutima waboongoka. ¹¹ Osalekelela kwendo kwamuntu ozitukumula kubwela pafupi naine. Osalekelela kwanja koipa kuniyendesha ine. ¹² Kuja ochita voipa bagwa; bagwesewa, ndipo sibakwanisa kuimila.

Chapter 37

Salimo ya Davide. ¹ Osakalipisiwe chifukwa chabochita voipa; Osakubwila vochita va bamene sibolungama. ² Chifukwa manje manje bazayuma monga uzu na kufota monga msipu. ³ Kulupilila Yehova na kuchita vabwino; khala mumalo na kudye mokulupilika. ⁴ Ndipo uzikodwelese iwe muli Yehova, ndipo azakupasa zofuna za mtima wako. ⁵ Peleka njila zako kuli Yehova; mukulupilile eve, na azakuchitila iwe. ⁶ Azaonesa chilungamo chako monga muzuba, na kusalakwa kwako ngati mumazulo. ⁷ Khala zii pameso pa Yehova ndipo umuyembekezele bwino. Osakalipa ngati winangu achita bwino muvamene achita, kapena akapanga vintu voipa. ⁸ Osakalipa na kuvela kuipa. Osadandaula. Ivi vimabweleselako mavuto. ⁹ Bochita voipa azaduliwa, koma bamene bayembekezela Yehova bazalandila ziko yapasi. ¹⁰ Mukantawi kang'ono muntu oipa azasoba; uzayang'ana malo yake, koma aza yenda. ¹¹ Koma bozichepesa bazatenga ziko yapasi ndipo bazakondwela mukuyenda pasongolo kwabo. ¹² Boipa bapanga mapulani boipa ku bolungama, ndipo akukukutula meno chifukwa cha bukali. ¹³ Mbuye amuseka, pakuti aona kuti siku yake ibwela; ¹⁴ Boipa asolola malupanga yabo ndipo bapindamula mauta yao kuti bagwese bochitikiziwa nabo vutika, kuti bapaye blungama. ¹⁵ Malupanga yao yazalasa mitima yao, na mauta yao yazathyolewa. ¹⁶ Chilibwino ving'ono vabolungama kuchila vambili va bantu boipa bambili. ¹⁷ Pakuti manja ya boipa yadzathyolewa, koma Yehova asamalila bolungama. ¹⁸ Yehova amayang'anila bangwiro siku na siku, ndipo cholowa chao chizakhala muyayaya. ¹⁹ Sibaza vela nsoni panthawi yoipa. Njala ikabwela, bazakhala na vakudya vambili. ²⁰ Koma bantu boipa bazawonongeka. Badani ba Yehova bazakhala monga ulemlelo wa mauzu; bazadyewa na kusoba mu chusi. ²¹ Muntu oipa amabweleka, koma samabweza, koma olungama apasa bwino. ²² Bodalisiwa na Mulungu bazalandila malo; bamene bali botembelelewa ndiye bazajubiwa. ²³ Nimuli Yehova mwamene mayendedwe ya muntu yakazikisiwa, Muntu wamene njila yake ili yotamandika pameso pa Mulungu. ²⁴ Olo kuti azezeleka, sazagwa, pakuti Yehova wamugwila na kwaanja yake. ²⁵ Neze mung'ono, manje nakula; Nikalibe kuonapo muntu olungama kusiyiwa, kapena bana bake kupempha vakudya. ²⁶ Siku yonse alina chifundo, naku kongolesa, na bana bake bakhala daliso. ²⁷ Siya zoipa, na kuta cilungamo; ndipo uzakhala otetezewa muyayaya. ²⁸ Pakuti Yehova akonda chilungamo, ndipo satailila okhulupilika bake. Basungiwa muyayaya, koma bobadwa mumbuyo mwa boipa. ²⁹ Olungama bazalandila ziko yapansi, nakukhala mwame muja muyayaya. ³⁰ Kamwa ka muntu olungama kamakamba vanzelu, nakuikilako chilungamo. ³¹ Lamulo ya Mulungu wake ili mumtima mwake; mendo yake sizatelele. ³² Muntu oipa amatamba olungama na kufuna kumupaya. ³³ Yehova sazamusiya mumanja mwa oipa uyo kapena kumukalipila poweluziwa. ³⁴ Yembekezela Yehova na kusunga njila zake, ndipo nyamula iwe pamwamba kutenge ziko. Uzaona pamene boipa bajubiwa. ³⁵ Naonapo muntu oipa ndi oyofya kufalika ngati mtengo wobilibila muthaka yake. ³⁶ Koma pamene ninapitilako futi, eve pezelibe. Ninamufunafuna, koma sanapezeke. ³⁷ Onese-seni muntu wangwilo, ndipo muzindikile bolungama; kuli sogolo yabwino ku muntu wantendele. ³⁸ Bochimwa bazawonongewa mofikapo; sogolo ya oipa niyojubiwa. ³⁹ Chipulumuso cha olungama chichokela kuli Yehova; amabateteza muntawi ya masauso. ⁴⁰ Yehova amabatandiza na kubapulumusa. Amabachosa kuli bantu boipa na kubapulumusa chifukwa bamatabila kuli eve.

Chapter 38

Salimo ya Davide, yo bwelesa kukumbuka. ¹ Yehova, musanizuzule na ukali wanu; musanilanga muukali wanu. ² Pakuti mivi yanu yanilasa, ndipo kwaanja yanu inipanikiza. ³ Thupi yanga yonse yadwala chifukwa chaukali wanu; mumafupa yanga mulibe moyo chifukwa cha machimo yanga. ⁴ Pakuti machimo yanga yanipakila; ndipo yanilemela manigi ine. ⁵ Vilonda vanga vaola ndipo vinunka chifukwa cha kupusa kwa machimo yanga. ⁶ Nimadyakiwa na kunyozewa siku na siku; Nimayenda kulila siku yonse. ⁷ Pakuti mukati mwanga, mwazula nakuyaka; mubili wanga siulibwino. ⁸ Nazizila ndipo naphwanyiswa ndintu; Nikulila chifukwa mtima wanga ubaba. ⁹ Mbuye, muziba wamene mtima wanga ufuna, Na kulila kwanga sikobisika kuli imwe. ¹⁰ Mtima wanga ugunda, mphamvu zanga zasila, na meso yanga yafota. ¹¹ Bazanga na benangu sibanifuna chifukwa cha chamwamene nilili; banasi banga bama imilila patali. ¹² Bamene basakila moyo wanga anichela misampha; Bamene bafuna kuipa pali ine bakamba mau yoipa ndipo bamakamba mau yonama siku yonse. ¹³ Koma ine, nili ngati muntu alibe matfu, ndipo sinivela vilivose; Nili ngati muntu osaka ba wamene sakamba chili chonse. ¹⁴ Nili ngati muntu wamene savela ndipo alibe voyanka. ¹⁵ Zooni nizakuyembekezani, Yehova; Mbuye Mulungu wanga. ¹⁶ Nikamba ivi kuti badani banga basasangalale pali ine. Ngati mendo yanga yagwa, bazachita voipa kuli ine. ¹⁷ Chifukwa nili pakugwa, ndipo nili kuvela kubaba kosasila. ¹⁸ Nivomela kulakwa kwanga; Nili na nkhawa na chimo yanga. ¹⁹ Koma badani banga nibambili; bamene banizonda molakwika nibambili. ²⁰ Banibwezela kuipa mumalo mwa vabwino; banama pali ine olo nachita vabwino. ²¹ Musanisiye ine, Yehova; Mulungu wanga, musakhale kutali naine. ²² Bwelani musanga kunitandiza, Mbuye, ndimwepulumuso changa.

Chapter 39

Kuoyimba nyimbo mukulu, Yedutuni. Salimo ya Davide. ¹ Ninaganiza kuti, "Nizayanganisisa vamene nizamkamba kuti nisachimwe nalilime yanga. Nizavala pakamwa panga pameso pa muntu oipa." ² Ninakhala zii; Ninasunga mau yanga kukamba vili vonse olo vabwino, na kubaba kwanga kunakula. ³ Mtima wanga unapya; pamene ninaganiza pa ivi, unapya ngati mulilo. Ndipo ninakamba. ⁴ "Yehova, nizibiseni ine pamene moyo wanga uzasila na utali wa masiku yanga. Nlangizeni mwamene nilii ochepelako." ⁵ Onani, mwasandusa masiku yanga ngati m'lifupi ya kwanja yanga, ndipo masiku yakhala ngati yalibe kantu pameso panu; Ndithu, muntu aliyense ali ngati kufuza kamozi. Selah ⁶ Zoona, muntu aliyese amayenda ngati chinvinvili. Ndithu aliyese atamangila kupanga chuma ngakhale kuti saziba wamene azasala navo. ⁷ Manje, Mbuye, niyembekezela chiani? Imwe ndimwe chiyembekezo changa cheka. ⁸ Nipulumuseni ku machimo yanga; musanipange chitonzo cha chavipuba. ⁹ Nakhala zii nakamwa kanga sikangaseguke, chifukwa ndimwe mwachita. ¹⁰ Siyani kunichita; Nili ozuliwa na kuwomba kwa kwanja yanu. ¹¹ Pamene mulanga bantu chifukwa cha chimo, muma ononga vofuna vake ngati njenjete; Zoona, bantu bonse balibe kantu koma ntunzi. Selah ¹² Velani pempheo yanga, Yehova, niveleni ine; velani kulila kwanga! Musankale osavela, pakuti nili ngati mlendo kuli imwe, mobisama ngati makolo yanga yonse. ¹³ Pindamulani meso yanu kuti nisekelele nafuti.

Chapter 41

Kwa musogoleli wa boyimba. Salmo ya Davida. ¹ Odalisika ni muntu wamene ama fakila nzelu kuli bo foka; mu masiku ya mavuto, Yehova azamupulumusa. ² Yehova azamusunga nakumusunga wa moyo, ndipo azankala wo dalisika pa ziko la pansi; Yehova sa zamupasila ku chifunilo chabadani bake. ³ Yehova azamutandiza pa kama ya mavuto, muzapanga kama yake ya matenda kunkala kama yamachiliso. ⁴ Nina kamba, "Yehova, ninvelele chifundo! Nipolese, chifukwa nachimwa." ⁵ Ba dani banga bakamba voipa pali ine, kukamba kuti, 'Niliti pamene azafa na zina yake kuwonongeka?' ⁶ Ngati mudani wanga abwela kuniwona, amakamba vintu vilibe nchito; mutima wake umafaka pamozi chiwonongeko changa cheka; akachok pali ine, amawuza benangu pali ivi. ⁷ Bonse bamene banizonda bama vwiya pali ine; pali ine bamafuna voipa. ⁸ Bamakamba kuti, "Matenda yoyipa yagwililila pali eve; manje kuti agona pansi, sazawuka nafuti." ⁹ Zoona, olo munzanga wanga wapafupi, wamene nichetekela, anadya mukate wanga, anyamula mendo yake pali ine. ¹⁰ Koma iwe, Yehova, ninvelele chifundo nakuninyamula kuti nibabwezelemo. ¹¹ Koma ichi niziba kuti usangalala muli ine, chifukwa badani banga sibawina pali ine. ¹² Kuli ine, mumani tandiza mu chilungamo changa nku nisunga pamenso yanu kwamuyayaya ¹³ Lekani Yehova, mulungu wa israeli atamandiwe kuchokela kumuyayaya kufikila kumuyayaya. Amen ndipo Amen.

Chapter 42

Kuli musogoleli wa boyimba. Maschil ya bana bamuna ba korah. ¹ Monga mwamene mbawala imafuna musinje wa manzi, ndiye mwamene nimakunvelela njota, mulungu. ² Nimanvela njota ya mulungu, ya mulungu wa moyo, niliti pamene nizabwela naku wonekela kuli iwe mulungu? ³ Misozi yanga inali chakudya changa muzuba na usiku, pamene ba dani banga banali kuniwuzwa lyonse kuti, "mulungu wako alikuti?" ⁴ Ivi vintu nimakumbuka pamene nimatila umoyo wanga: mwamene ninayenda na khamu naku basogolela ku nyumba ya mulungu na mau yachisangalalo nama tamando, ma gulu kusangalala chikondwelelo. ⁵ Nichani wagwada pansi, umoyo wanga? Nichani ukalipa mukwati mwanga, kulupilila muli mulungu, chifukwa nafuti niza mutamanda wamene ali chipulumuso changa. ⁶ Mulungu wanga, umoyo wanga unagwada mukati mwanga, mwaicho nimikumbukani mu nzelu kuchokela ku malo ya Yodani, kuchokela ku nsonga zitatu za lupili lwa Hermoni, naku chokela ku pili ya Mizar. ⁷ Manzi akuya amayitana kuya pa chongo cha kugwa kwa manzi anu; mafunde anu onse na mafunde yayenda pamwamba panga. ⁸ Ndipo Yehova azawuza chipangano chake chachilungamo mu ntawi yamuzuba; usiku nyimbo yake izankala naine, pempelo ku mulungu wa moyo wanga ⁹ Nizakamba kuli mulungu wanga, mwala wanga, "Nichani waniyibala? Nichani niyenda nilila chifukwa chachofyantiwa naba dani banga?" ¹⁰ Monga lupanga mumafupa yanga, ba dani banga bani zuzula, pamene baniwuzwa lyonse kuti, "Alikuti mulungu wako?" ¹¹ Nichani ugwada pansi, moyo wanga? Nichani ukalipa mukati mwanga? Kulupilila muli mulungu.

Chapter 43

¹ Niletele chilungamo, mulungu, naku chondelela mlandu wanga pali maziko yamene yalibe chilungamo. ² Pakuti ndiwe mulungu wa mpavu zanga. Nichani wanikana? Nichani niyenda mukulila chifukwa chakufyantiwa naba dani banga? ^{3 4} Oh, tuma nyali yako nachi lungamo chako, vilekeni vinisogolele. Vilekeni vinilete ku pili yanu yoyela naku mankalidwe yanu. Ndipo nizayenda pa guwa ya mulungu, kuli mulungu chisngalalo changa chachikulu. Nizakutamanda na zeze, mulungu, mulungu wanga. ⁵ Nichani ugwada pansu, moyo wanga? Nichani ukualipa mukati mwanga? Kulupilila muli mulungu, chifukwa nafuti nizamutamanda wamene alichipulumuso changa ndipo mulungu wanga.

Chapter 44

Kuli mukulu waboyimba. salmo yabana ba Korah. Mu maschil. ¹ Tanvela na matu yatu, mulungu, batate batu banatiwuza nchito zamene unachita mumasiku yawo, masiku yakudaala. ² Unapisha maziko nakwanja kwanja kwako, koma unashanga bantu batu; unavutisa batu, koma unamwazika bantu batu mumalo. ³ Chifukwa sibana landile malo yonkalamo yao kupitila mu lupanga lwao, kapena kwanja kwawo kubapulumusa; koma kwanja kwanu kwa zanja la manja, ndipo nyali ya mkope yako, chifukwa munabakondelani mtima. ⁴ Mulungu, ndiwe mfumu yanga; lamulila kupambana kwa Yakobo. ⁵ Kupitila muli iwe tizagwesa ba dani batu; kupitila muzina yako tiza baponda pansi, baja bonyamuka kususana naise. ⁶ Chifukwa siniza chetekela mu uta yanga, kapena lupanga yanga kunipulumusa. ⁷ Koma wati pulumusa kuchokela ku badani batu, nakuvensa nsoni bamene batizoonda. ⁸ Muli mulungu tizinvesa masiku yonse, ndipo tizawonga zikomo kuzina lanu kwamuyayaya. Selah ⁹ Koma manje watitaya naku tiletela manyazi, ndipo siuyenda panja nama gulu ya nkondo yatu. ¹⁰ Utilengesa ku taba badani batu; ndipo bamene batizoonda batitenga zofunka zao. ¹¹ Watipanga monga nkosa zifunika kupaya ndipo watimwazika pakati pamaziko. ¹² Wagulisa bantu bako pa chabe; sunachulise chuma chako pochita ichi. ¹³ Watipanga chizuzulo ku bantu bapafupi, onyozedwa naku sekewa kuli bo tizunguluka. ¹⁴ Watipanga chipongwepakati pamaziko, kunyang'anyisa mutu pakati pa bantu. ¹⁵ Masiku yonse manyazi yanga yali pali ine, na nsoni za nkope yanga zani vwinikila, ¹⁶ chifukwa cha mau ya wamene azuzula nakutukana, chifukwa cha badani naobwezela. ¹⁷ Zonse izi zabwela pali ise; ngakale sitinakuyibale kapena kuchita zaboza na chipangano chako. ¹⁸ Mitima yatu sinabwelele mumbuyo; mayendedwe yatu sanachoke munjila yako. ¹⁹ Koma watipwanya maningi mu malo ya mimbulu naku tivwinikila na chintuzi cha infa. ²⁰ Ngati tayibala zina ya mulungu watu kapena kutambusula manja yatu ku mulungu wachilendo, ²¹ sembe mulungu sanasakile? chifukwa aziba zinsinsi za mutima. ²² Zoona, chifukwa chako batipaya masiku yonse; tiwoneka monga nkosa zifinika kupaya. ²³ Ukani. nichani mugona, Ambuye? Nyamukani, musatitayilile kwamuyayaya. ²⁴ Nichani mubisa nkope yanu naku yibala kuvutika naku fyantiwa kwatu? ²⁵ Chifukwa tambila mu fumbi; ma tupi yatu yagwilila ku ziko ya pansi. ²⁶ Nyamuka kuti utitandize nakutiwombola pa chifukwa cha chipangano chako chokulupilika.

Chapter 45

Kuli musogoleli wa boyimba; Bonkala ku Shoshannim. Salmo ya bana ba Korah. Mu maschil. Nyibo yachikondi. ¹ Mutima wanga umasefuka pa nkani ya mushe; nizabelenga monveka mau yamene nalembela mfumu; lilimi lyanga nicholembela cha wolemba wokonzeka. ² Uliko mushe kuchila bana ba bantu; chisomo chatayiwa pa mulomo wako; mwaicho tiziba kuti mulungu akudalisa kwayayaya. ³ Ika lupanga lwako pambali, wampanvu, mu ulemelelo wanu na ukulu wanu. ⁴ Mu ukulu wanu nkwele mopambana chifukwa chaku kulupilika, kufasa na chilungamo; kwanja kwanu kwa zanja la manja kuza ku punzisa zintu zoyofwa. ⁵ Mivi yanu niyonolewa; bantu bamagwa pansu panu; mivi yanu ili mumitima yaba dani ba mfumu. ⁶ Mupando wanu wachifumu, ambuye, niwamuyayaya; ndodo yachiweluzo ni ndodo ya ufumu wanu. ⁷ Mwakonda chilungamo nakuzonda voipa; mwaicho mulungu, mulungu wanu, amizozeka na mafuta yachisangalalo kuchila banzanu. ⁸ Vovala vanu vonse vinunkila monga mure, aloye, kasiya; kuchokela munyumba yachifumu zida za nyanga zakukondwelesa. ⁹ Bana bakazi ba mfumu bali pakati pabakazi bolemekezeka; pa kwanja kwanu kwa zanja la manja kuimilila mukazi wa mfumu ovala golide za opiya. ¹⁰ Nvelani, bana bakazi, ganizilani nakuyika matu yanu; musaibale bantu banu na nyumba yaba tate banu. ¹¹ Mu njila iyi mfumu azakafuna umushe wako; ni mbuye wako; mulemekeze. ¹² Mwana mukazi wa Tyre azamkalapo na mpaso; bolemela pakati pa bantu bazaka papata kuti mubachitile zabwino. ¹³ Mwana mukazi wachifumu mu nyumba ya mfumu ni waulemelelo; vovala vake nivopangiwa na golide. ¹⁴ Azasogolelewa kuli mfumu mu dilesi losokedwa na nsalu; anamwali, banzake bamene bamukonka, bazaletewa kuli iwe. ¹⁵ Bazasogolelewa na chisangalalo naku kondwela; bazangena mu nyumba ya mfumu. ¹⁶ Mu malo ya atate banu kuzankala bana banu, bamene muzapanga akalonga mu ziko ya pansu yonse. ¹⁷ Niza ka panga zina lako kukumbukiwa mumibado yonse; mwaicho bantu baza kaomga zikomo kwamuyayaya.

Chapter 46

Kuli musogoleli wa boyimba. salmo yabana ba korah; bonkala ku Alamoti. Nyimbo. ¹ Mulungu nichotabila chatu na mpavwu, wamene amankalako pantawi ya mavwuto. ² Mwaicho sitiza yopa, ngakale ziko ya pansi inga chinje, ngakale mapili yanga nyang'anye mumitima ya nyanja, ³ ngakale manzi yake yawulumu na ukali, ndipo ngakale mapili yanjenjema na kutupaa kwawo. Selah. ⁴ Kuli mumana wamene misinje yake ipanga muzinda wa mulungu kusangalala, malo yoyela amene amankala wamumwambamwamba. ⁵ Mulungu alipakati pake; saza vendezewa; mulungu azamutandiza, ndipo azachita vamene pakucha kwaku seni. ⁶ Maziko alina ukali ndipo umfumu ananyang'anyisiwa; ananyamula mau yake, ndipo ziko ya pansi inasungunuka. ⁷ Yehova wamakamu alinaise; mulungu wa Yakobo ni chitabilo chatu. Selah ⁸ Bwelani, onani machitidwe ya Yehova, chiwonongeko chamene achita pa ziko ya pansi. ⁹ Apanga nkondo kusila kosilila ziko ya pansi; ama pwanja uta nakujuba mkonod muvi dunswa dunswa; amajuba vi chingilizo. ¹⁰ Nkalani osimikiza ndipo muzaziba kuti ndine mulungu; nizakwezekewa bakati pama ziko; nizakwezekewa pa ziko ya pansi. ¹¹ Yehova wamakamu alinaise; mulungu wa Yakobo ni chotabila chatu. Selah

Chapter 47

Kuli musogoleli waboyimba. Salmo ya bana ba Korah. ¹ Wombani manja yanu, imwe bantu bonse; fuulani kuli ambuye na mau yachipambano. Pakuti ² Yehova wamumwambamwamba niwoyofya; nimfumu ikulu muziko ya pansi yonse. ³ Amagonjesa bantu pansi patu na maziko pansi pa mendo yatu. ⁴ Amatisankila cholowa chatu, ulemelelo wa Yakobo wamene nali kukonda. Selah ⁵ mulungu ayenda mumwamba naku punda, Yehova nakulila kwa lipenga. ⁶ Imbani matamando kuli mulungu, imbani matamando; imbani matamando kuli mfumu yatu, imbani matamando. ⁷ Chifukwa mulungu ni mfumu muziko ya pansi yonse; imbani matamando mozindikila. ⁸ Mulungu alamulila pa maziko; mulungu ankala pamupando wake woyela. ⁹ Bana ba mfumu ba bantu bankala pamozi kuli bantu ba mulugu wa Abraham; chifukwa chichingilizo chabantu nicha mulungu; niwonyamuliwa kwambili.

Chapter 48

Nyimbo; salmo yaban ba korah. ¹ Mukulu ni Yehova ndipo ayenela kutamanda kwambiri, mu muzinda wa mulungu watu pa lupili yake yoyela. ² Wokongola papili itali, chisangalalo cha ziko yapansi yonse, ni lupili ya ziyoni, kumbali kwa kumpoto, muzinda wa nfumu ikulu. ³ Mulungu azizibisa mu nyumba yamfumu yake kuti ni chitabilamo. ⁴ Chifukwa, Onani, mfumu zankala pamozi; bapita pamozi. ⁵ Banaziwonela, ndipo banasangalala; bana yopa, ndipo banataba. ⁶ Kunjenjema kunabagwila, kubaba monga mukazi wamene abala. ⁷ Na mpepo yakumawa upwanya zombo zaku Tarshishi. ⁸ Mwamene tanvelela, ndiye mwamene tawonela mumuzinda wa Yehovah wamakamu, mu muzinda wa mulungu watu; mulungu azatiyimika kwamuyayaya. selah ⁹ Taganizilapo pali chipangano chako chokulupilika, mulungu, pakati pa kachisi yako. ¹⁰ Monga mwamene ilili zina yanu, mulungu, ndiye mwamene yalili matamando kufikila kosilila chalo; kwanja kwanu kwa zanja la manja niyozula chilungamo. ¹¹ Lekani lupili ya Ziyoni isangalale, lekani bana bakazi ba Yuda basangalale chifukwa cha malamulo yanu yolungama. ¹² Yenda mozunguluka lupili ya Ziyoni, zinguluka; penda sanja zake, ¹³ yanganisisa zipupa zake, ndipo yangana nyumba za mfumu zake chakuti ungawuze mibado yokonkapo. ¹⁴ Chifukwa uyu mulungu ni mulungu watu kwamuyayaya; azamkala mulangizi kufikila pokufa

Chapter 49

Kuli musogoleli waboyimba. Salmo ya bana ba Korah. ¹ Nvelani ichi, imwe bantu bonse; nvelani, bonse bonkala muchalo, ² bonse bapansi na pamwamba, bolemela nabosauka bonse. ³ Kamwa izakamba nzelu ndipo ku sinkasinka kwa mutima wanga kuzankala kuzindikila. ⁴ Nizachela kutu yanga kuli fanizo; nizayamba fanizo yanga na zeze. ⁵ Nichani niyope masiku yoyipa, pamene kusaweruzika kundizungulila? ⁶ Nichani niyope abo bamene bachetekela muli chuma chao nakuzivensa pali chuma chao? ⁷ Chizibika kuti kulibe wamene angawombole bale wake kapena kulipila mulungu pali eve, ⁸ chifukwa kuwombola munyu nichodula, ndipo kulibe angatilipilile nkongole yatu. ⁹ Kulibe angankale wamoyo kwamuyayaya chakuti tupi yake isawole. ¹⁰ Chifukwa azawola. Bamuna banzeli bamafa; balibe nzelu na wopanda nzelu bamawongeka nakusiya chuma chawo kuli benangu. ¹¹ Maganizo yawo yamukati niyakuti ma banja yawo yazakonkaniza kwamuyayaya, na malo yamene bankala, ku mi bado yonse; bamayitana malo yao zina yao. ¹² Koma muntu, alina chuma, samasala wamoyo; alimonga nyama yamunsanga yamene imafa. ¹³ Ichi, iyi njila, niwupuba wao; ndipo kuchoka beve, bantu bavomekeza mau yao. Selah ¹⁴ Monga nkosa basankiwa kuli manda, na infa izankala wobayembela. Bolungama baza balamulila kuseni, ndipo matupi yao yazadyewa na manda, kulibe malo yao yonkala. ¹⁵ Koma mulungu azawombola moyo wanga kuchokela ku mpavwu za manda; azanilandila. Selah ¹⁶ Musayope ngati umozi alemela, ndipo ulemelelo wa nyumba yake uzapaka. ¹⁷ Chifukwa akafa sazatenga chilichonse; ulemelelo wake suzamukonka. ¹⁸ Anadalisa moyo wake pamene anali wa moyo- ndipo bantu bakutamanda ngati uzinkalila- ¹⁹ azayenda kumibado yaba tate bake ndipo sabazawona nyali nafuti. ²⁰ Wamene ali na chuma koma alibe nzelu alimonga nyama zamene ziwonongeka.

Chapter 50

¹ Salmo ya Asafi. Wampavu, mulungu, Yehova, akamba nakuyitana ziko ya pansi kuchokela kwamene inyamukila zuba kufikila kwamene imbilila. ² Kuchokela mu Ziyoni, ungwiro wokongola, mulungu ayasha. ³ Mulungu watu abwela ndipo sasiya kukamba; mulilo uwononga pasogolo pake, ndipo kuli chimpepo pali eve. ⁴ Amaitana kumwamba na pa ziko ya pansi chakuti alamulile bantu bake: ⁵ "ikani bolungama banga pamozi kuli ine, abo banapanga chipangano naine na zopeleka." ⁶ Myamba izakakamba chilungamo chake, chifukwa mulungu pali eka niwoweruza. Selah ⁷ "Nvelani, bantu banga, ndipo nizakamba; ndine mulungu, mulungu wanu." ⁸ Siniza mizuzula pali zipeleka zanu; zopeleka zanu zo shoka lyonse zili pali ine. ⁹ Sinizatenga ng'ombe imuna munyumba yanu, kapena mbuzi imuna mumakola anu. ¹⁰ Chifukwa nyama yonse munsanga niyanga, na ng'ombe pama pili yali sauzandi. ¹¹ Niziba tunyomi twamupili, vinyama vamunsanga nivanga. ¹² Ngati nenze nanjala, sembe sininamiuzeni; chifukwa chalo nichanga, na zonse zilimo. ¹³ kuti nadya nyama ya ng'ombe kapena kumwa gazi ya mbuzi?

¹⁴ Pasani kuli mulungu chopeleka cho onga zikomo, nakulipila lumbilo yanu kuli wakumwambamwamba. ¹⁵ Itana pali ine mumasiku ya mavuto; nizakupulumusani, ndipo muzanipasa ulemelelo." ¹⁶ Koma kuli boipa mulungu akamba, "mucita chani pali kukambilila malamulo yanga, kuti mwatenga chipangano changa mukamwa mwanu, ¹⁷ chifukwa muzonda chilungamo nakutaya mau yanga? ¹⁸ Mukawona kawalala, mumavomela neyeve; mumapezeka kuli bamene bachita chigololo.

¹⁹ Mumapasa kamwa yanu kuli voipa, na lulimi yanu kuli chinyengo. ²⁰ Mumankala nakukamba pali mulongo wanu; mumakamba pali mwana wa amai banu. ²¹ Mwachita vintu ivi, koma sinina kambe chili chonse, ndipo muganiza monga nili monga imwe. Koma nizamizuzula naku mileta pamwamba, pamenso yanu, vintu vonse vamene mwachita. ²² Viyanganisise, imwe bamene muyibala mulungu, nizaming'ambani muvidunswadunswa, ndipo sikuzabwela ali yense kumitandizani! ²³ Wamene apasa nsembe yotokoza anitamanda, ndipo aliyense wamene apanga njila zake mofunikila niza mulangiza chipulumuso cha mulungu."

Chapter 51

¹ Nichitileni chifundo ine, Mulungu, chifukwa chachipangano chokulupilika chanu; chifukwa cha kuchukula zochita zachifundo zanu, chosani zolakwa zanga. ² Nisambikeni bwinobwino kuma chimo yanga naku nichosa choyipa changa. ³ Pakuti niziba zolakwa zanga, na chimo yanga imankhala pali ine nthawi zonse. ⁴ Mosusa imwe, imwe chabe mweka, nakulakwilani nakuchita zonyansa pamanso panu; mwalungasiwa pamene mukakamba; ndimwe opanda cholakwa pamene muweruza. ⁵ Onani, ine ninabadwa muchimo ; posankhalisa bamayi banga bananitenga pakati, ninali muchimo. ⁶ Onani, mumafuna kukhulupilika mukati mwayine; ndipo muma niphunzisa nzelu mumalo yobisika mukati. ⁷ Niyeleseni na hisope, ndipo nizankhala oyela; nisambikeni ine nizankhala choyela kuchila matalala. ⁸ Lekani ni mvele kusangalala na kumvela bwino pakuti mabonzo yamene mwapwana muli ine yasangalale. ⁹ Bisani nkhope yanu kumachimo yanga na kuchosa zoyipa zonse zanga. ¹⁰ Pangani muli ine mutima woyela, na kukonza muzimu wa zooni mukati mwa ine. ¹¹ Osanithamangisa pamanso panu, osatenga Muzimu Oyela muli ine. ¹² Bwezelani kwa ine chisangalalo cha chipulumuso chanu, nakunichilikiza na muzimu wololela. ¹³ Ndipo ine nizaphunzisa olakwila njila yanu, na bochimwa bazatembenuka. ¹⁴ Nikululukileni pokesa mwazi, Mulungu wa chipulumuso changa, ndipo nizapunda mosangalala pachilungamo chanu. ¹⁵ Ambuye, segulani milomo yanga, nakamwa kanga kaonese matamando yanu. ¹⁶ Pakuti imwe simumakondwela mu nsembe, kapena ningapase ; imwe mulibe chisangalalo munsembe zopsereza. ¹⁷ Nsembe ya Ambuye ni muzimu yopwanika. Imwe, Ambuye, mutima wopwanika na wolakwa simuza unyozwa. ¹⁸ Chitani chabwino muchisangalalo chanu ku Zioni; mangani vipupa va mu Jerusalemu. ¹⁹ Ndiye pamene muza sangalala munsembe ya chilungamo, mu nsembe zopsereza na zonse nsembe zopsereza; ndipo banthu bonse bazapeleka ng'ombe zimuna pa guwa.

Chapter 52

¹ Kodi nichani uzitukumuza pakuleta musokonezo, iwe mwamuna wamphamvu? Chipangano chokulupilika cha Mulungu chimabwela pa nthawi zonse. ² Lilime yanu imapanga zowononga monga kaleza konola, kugwila nchito mwachinyengo. ³ Mukonda kuchita zoyipa kuchila zabwino na kunama kuchila kukamba chilungamo. Selah ⁴ Imwe mukonda mau yamene yamakumeza bena, iwe lilime yachiyengo. ⁵ Mulungu azakami wonongani imwe muyayaya; azakamithengani nakukudulani mu hema mwako na kukuchosani muziko ya amoyo. Selah ⁶ Olungama azaona nakunkhala namanta; beve bazamuseka eve nakukamba kuti, ⁷ " Onani, uyu ndiye mwamuna wamene sanapange Mulungu wake kumuchingiliza, koma iye anakulupilila muchuma cake chambili, ndipo anali wamphamvu pamene anali kuwononga banthu bena." ⁸ Koma ine, nili monga mutengo wa azitona yobiliwila mu nyumba ya Mulungu; Nizafaka chikulupililo chachipangano chokulupilika ya Mulungu mu muyayaya na muyayaya. ⁹ Niza kuthamandani muyayaya pavinthu vamene mwachita. Niza yembekeza pa zina yanu, chifukwa ni yabwino, pamanso pa okulupilika banu.

Chapter 53

¹ Chipuba chimakamba mutima mwake kuti, " kulibe Mulungu." Nibachiyengo nakuchita machimo yoyansa; kulibe na umozi amene amachita zabwino. ² Mulungu amaona kuchokela kumwamba pa bana ba banthu kuti awone ngati pali bamene bamvela, bamene bamusakila iye. ³ Bonse bapatuka. Pamozi ba nkhalabachiyengo. Kulibe umozi wamene achita chabwino, ngankhale umozi. ⁴ Kodi bamene bamachita zoyipa balibe nzelu-bamene bamadya banthu banga monga ngati bakudya bledi ndiponso sibamayitana pali Mulungu ? ⁵ Balipo , mumanta yakulu, pamene kunalibe chilichonse chobayofya; pakuti Mulungu azamwaza mafupa ya bamene bazinga imwe; imwe muzabafaka manyanzi , chifukwa Mulungu abakana . ⁶ O, chipulumuso chamene ichi cha israeli chingabwele kuchokela ku Ziyoni ! Pamene Mulungu abwelesa banthu bake kuchokela mubukapolo, ndiye Yacobo azasangala na Israeli azakondwela !

Chapter 54

¹ Ni mpulumuseni, Mulungu, na zina yanu, niweluzeni ine mumphamvu zanu. ² Mvelani mpempelo yanga, Mulungu; mvelani ku mau yamene yalimu kamwa mwanga. ³ Balendo baniwukila motsusana naine, bamuna opanda chifundo banifunafuna kuti banipaye in; sibanaike Mulungu pamanso pawo. Selah ⁴ Onani, Mulungu ndiye mthandizi wanga; Ambuye ndiye amanilimbikisa ine. ⁵ Azabwezela ba ndani banga nazoyipa; mukulupilika kwanu, muba wononge ! ⁶ Ni zapeleka ufulu kuli imwe; niza thamanda zina yanu, Yehova, chifukwa ni yabwino. ⁷ Pakuti mwani mpulumusa kuchokela kuba ndani banga.

Chapter 72

Salmo ya Solomoni. ¹ Pasani mfumu maweluzo yolungama yanu, Mulungu, chilungamo chanu kuli mwana wa mfumu. ² Aweluze bantu banu mwachilungamo, na bosauka banu na chilungamo. ³ Mapili yabwelese mtendele ku bantu; ma chulu yabale chilungamo. ⁴ Aweluze bosauka ba bantu; apulumuse bana ba bosauka, na kupwanya bosausa. ⁵ Bakulemekezeni pamene zuwa ikali kubala, pamene mwezi unkala kupita mumibadwo bonse. ⁶ Aseluke monga mvula pamauzu yojubiwa, monga mvula yotilila ziko ya pansi. ⁷ Mu masiku yake yolungama yazikula bwino, mtendele unkale bochuluka kufikila ntawi kuti mwezi kulibe. ⁸ Ankale na ulamulilo kuyambila kunyanja kufikila kunyanja, na kuyambiaa ku Musinje kufikila malekezelo ya ziko ya pansi. ⁹ Bantu bonkala muchipululu bagwade pamenso pake; badanib bake bamyangute fumbi. ¹⁰ Mafumu ya Tarisi na visumbu bazipeleka musonko; Mafumu ya ku Seba na Seba bazipeleka mphaso. ¹¹ Inde, mafumu yonse yagwadile pamenso pake; mitundu yonse bamtumikile. ¹² Pakuti eve amatandiza waumpawi bolila na bosauka bamene balibe obatandizi wina. ¹³ Amanvela chisoni bantu bosauka na bosoba, ndipo amapulumusayo moyo wa bantu bovutika. ¹⁴ Amaombola miyobo yabo ku dyakililiwa na ndeo; ndipo magazzi yabo niyamtengo wapatali mu menso wake. ¹⁵ Ankale na moyo! Bamupase golide ya Sheba. Bantu bamupmemphelele ntawi zonse; Mulungu amudalise siku yonse. ¹⁶ Paziko ya pansi pankale mbeu yochuluka; Vokolola vawo pa nsonga za mapiri. vipaso vake vinkale ngati Lebano; banthu bakule mu minzi ngati mauzu ya kusanga. ¹⁷ Zina yake inkhale ilibe kosata; zina yake inkhale ipitilize masiku yonse yazuwa; bantu badalisiwe mwa eve; bamitundu bonse bamuitana odalisika. ¹⁸ Yehova Mulungu, Mulungu wa Isiraeli, adalisike, wamene ekha amachita vodabwisa. ¹⁹ Zina yake yaulemelelo idalisike kosata, ndipo ziko yonse yapansi izale na ulemelelo wake. ²⁰ Amene Amene. Mapempelo ya Davide mwana wa Jese yasila.

Chapter 73

Salimo ya Asafu. ¹ Zoona, Mulungu niwabwino kuli Israeli, kuli beve ba mitima yoyela. ² Koma ine, mendo yanga yanafuna kutelela; mendo yanga kunasala pang'ono kuti nigwe pansi panga, ³ pakuti ninachitila nsanje bozikweza, pamene ninaona ubwino wa boipa. ⁴ Chifukwa sibana nvelepo kubaba mpaka infa, koma balina mpamvu naku kuta. ⁵ Nibomasuka ku mabvuto ya bantu bena; Sibavutika monga bantu bena. ⁶ Kuzikweza kubakongolesa monga mkanda pamukosi; ndeo ibavaliika monga mukanjo. ⁷ Kuchokela mu umpofu monga uyu mumachokela chimo; maganizo yoipa yapita mu mitima mwabo. ⁸ Banyoza naku kamba voipa; mukuzikuza kwabo bayopesa kudyakililiwa. ⁹ Kamwa kabo kayikiwa kumwamba, na lulime wabo iyenda paziko ya pansi. ¹⁰ Chifukwa chaichi bantu bake batembenukila ku beve, ndipo manzi yambili yasila. ¹¹ Bakamba "Ushe Mulungu akuziba bwanji? Mwati kuli Wapamwambamwamba kuli kuziwa?" ¹² Zindikilani: bantu aba ni boipa; ntawi zonse bamankala bosasamala, kunkala bolemela naku lemelelatu. ¹³ Zoona, nachingiliiza mutima wanga pachabe na kusamba mu manja mosalakwa. ¹⁴ Pakuti siku yonse nasausiwa na kulangiwa kuseni kulikonse. ¹⁵ Sembe nina kamba, "Nizakamba ivi," sembenina lekele bamubadwo uno wa bana banu. ¹⁶ Ngakhale kuti ninayesesa kunvesa vinthu vamene ivi, vinali vovuta kwambili kuli ine. ¹⁷ Ndipo nina ngena mu malo yopatulika ya Mulungu ndipo ninazindikila vamene vinabachitikila. ¹⁸ Zoona munabaika mu malo yotelela; mubagwesa ku chionongeko. ¹⁹ Mwamene beve bankalila chipululu mu kampindi! Babwela kumapeto ndipo basiliziwa mu voipa voyofya. ²⁰ Bankala ngati chiloto muntu akauka; Ambuye, imwe simuza nganiza vili vonse pali maloto aya. ²¹ Pakuti mtima wanga unali obaba, ndipo nichitwa maningi. ²² Ninali osaziba na opanda nzelu; Ninali ngati nyama yopusa pamenso panu. ²³ Koma ine nili na imwe ntawi zonse; mugwila kwanja yanga ya manja. ²⁴ Muzanisogolela na malangizo yanu ndipo pambuyo pake muzanilandila ku ulemelelo wanu. ²⁵ Nili na ndani kumwamba koma imwe? Palibe wina pa ziko ya pansi wamene nifuna koma inu; ²⁶ Tupi yanga na mtima wanga zifooka, koma Mulungu ndiye mpamvu ya mtima wanga na gabo yanga kosata. ²⁷ Baja bamene bali kutali na imwe bazaonongeka; muzaononga bonse bokusakulupilika kwa imwe. ²⁸ Koma ine, chamene nifunika kuchita niku bwela kuli Mulungu. Napanga Ambuye Yehova kunkala potabilapo panga. Niza kamba pa nchito zanu zonse.

Chapter 74

Nyimbo ya Asafu. ¹ Mulungu, mwatikana kosata? Chifukwa chani ukali wanu watishoka ise nkosa za busa panu? ² Kumbukilani bantu banu, bamene munagula kale, mutundu wamnee munaombola kuti inkale cholowa chanu, na pili ya Ziyoni, kwamene munkala. ³ Bwelani muzaone mabwinja yokwana, voipa vonse vamene mudani achita mu malo yoyela. ⁴ Badani banu banauluma pakati pa malo yanu yoikika; banaika ndembela zabo za nkondo. ⁵ Banatyola nkwangwa ngati mu nkalango yowilila. ⁶ Banapwanya naku pwanja volemba vonse; banavityola na nkwangwa na nyundo. ⁷ Banayasa malo yanu yopatulika; banaipisa ponkala imwe, nakugwesa pansi. ⁸ Banakamba mu mitima mwabo, "Tizaononga vonse." Banashoka malo yanu yonse yokumanila mu ziko. ⁹ Sitiona futi mazidinkilo; palibe futi mneneli, ndipo palibe aliyense mwa ife aziba kuti ivi vizachitika mpaka liti. ¹⁰ Mpaka liti, Mulungu, mdani azakunyoza? Kodi mdani azachitila mwano zina yanu kosata? ¹¹ Bwanji mubweza kwanja yanu, kwanja yanu ya manja? Chosani kwanja yanu ya manja pachovala chanu na kuwawononga. ¹² Koma Mulungu wankala mfumu yanga kuyambila kalekale, kupulumusa ziko ya pansi. ¹³ Munagaba nyanja na mpamvu zanu; munapwanya mitu ya vilombo va m'nyanja. ¹⁴ Munapwanya mitu yaba Leviatani; munamudyesa kwa okhala m'chipululu. ¹⁵ Munatyola bakasupe na misinje; munayumisa misinje yoyenda. ¹⁶ Siku ni yanu, na usiku niwanu futi; mumayika zuwa na mwezi pamalo yake. ¹⁷ Munaika malile yonse ya ziko ya pansi; munapanga zinja na zinja. ¹⁸ Kumbukilani kuti mdani wakunyoza imwe Yehova, na kuti bantu bopusa banyoza zina yanu. ¹⁹ Musapeleke moyo wa nkunda yanu kwa chilombo. Musaibale moyo wa bantu banu bosausiwa. ²⁰ Kumbukilani pangano yanu, pakuti madela yamdima ya ziko ya pansi pali ndeo ikulu. ²¹ Musabweze bosausiwa na manyazi; bovutika na bosausiwa balemekeze zina yanu. ²² Ukani, Mulungu; teteza ulemu wako; kumbukila mwamene visilu vimakutana chipongwe siku yonse. ²³ Musaibale mau ya badani banu kapena phokoso ya bantu bamene bakunyoza mosalekeza.

Chapter 75

Kwa boimba wamkulu; ku Al-Tasheti. Salimo ya Asafu, nyimbo. ¹ Tikuyamikani, Mulungu; tiyamika, pakuti mwaonesha mfeshi yanu; bantu bakamba nchito zodabwisa zanu. ² Pa nthawi yoikika nizaweluza mwachilungamo. ³ Ngankale ziko ya pansi izagwedezeke na bonse bonklamo, Ine nizalimbisa ma pilala ya ziko ya pansi. Selah ⁴ Ninakamba kuli bozi nvela, "Musazitukumule," na kwa boipa, "Osakweza nyanga. ⁵ Musakweze nyanga yanu pamwamba; osakamba na mukosi yachipongwe. ⁶ Sikuchokela kumaba kapena kumazulo, ndipo kukweza sikuchokela kuchipululu. ⁷ Koma Mulungu ndiye oweluza; amabweza pansi nakukwezeka pamwamba. ⁸ Pakuti Yehova agwila mukwanja yake chiko cha vinyu wamphumphu, yosankaniza na vonunkila, nakumutilila eve. zoonza boipa bonse ba paziko yapansi bazamwa mpaka to silizila. ⁹ Koma nizakamba kosalekeza vamene unacita; Nizaimba matamando ya Mulungu wa Yakobo. ¹⁰ Akamba: "Nizajuba nyanga zonse za boipa, koma nyanga za bolungama zizakwezewa.

Chapter 76

Kuli boimba wamkulu, na zisakasa. Salimo ya Asafu. Nyimbo. ¹ Mulungu azizibisa mu Yuda; zina yake ni yayikulu mu Israeli. ² Chihema chake chili ku Salemu; malo yake yonkala mu Ziyoni. ³ Kwamene uku anatyola mivi ya uta, lupanga, na zida zina zankondo. Selah ⁴ Muwala bwino nakuonesa ulemelelo wanu, pamene musika kuchokela kumapili, kwamene munapaya bantu. ⁵ Bolimba mtima banapokewa katundu; banagona tulo. Bankondo bonse banali bopanda chochita. ⁶ Pakuzuzula kwanu, Mulungu wa Yakobo, bokwelapo na kavalo banagona tulo. ⁷ Imwe, zooni imwe, muyenela kuyopewa; azaima pamenso panu ndani pamene mwakwiya? ⁸ Munamvekesa chiweluzo chanu kuchokela kumwamba; ziko ya pansi inachita manta na kunkala chete, ⁹ pamene munauka imwe, Mulungu, kuti muweluze, na kupulumusa bosausiwa bonse pa paziko ya pansi. Selah ¹⁰ Zooni chiweluzo chanu chaukali bantu chizaleta matamando kuli imwe; muzimangilila mu chuuno na chosala cha ukali wanu. ¹¹ Pangani lonjezo kuli Yehova Mulungu wanu nakuyi sunga. Bonse bomuzungulila babwelese mphatso kuli eve wamene ayenela kuyopewa. ¹² Ajuba mzimu wa bakalonga; bamamuyopa mafumu ya ziko ya pansi.

Chapter 77

¹ Nizaitana na liwi yanga kuli Mulungu; nizaitana liwi yanga kuli Mulungu, ndipo Mulungu wanga azaninvela ² Siku ya masauso yanga ninafuna Yehova; usiku ninatambulula manja yanga, ndipo siyanaleme. Moyo wanga unakana kutontozewa. ³ Ninaganiza za Mulungu pobuwula; Ninaganiza za eve pamene ninali kukomoka. Selah ⁴ Munanisegula menso yanga; Ninavutika kukamba. ⁵ Ninaganizila za masiku yakudala, ntawi zakudala. ⁶ Usiku ninakumbukila nyimbo yamene ninaimba ntawi imozi. Ninaganiza mosamala nikuyesa kunvesesa chamene chinachitika. ⁷ kodi Yehova azanikana muyaya? Mwati azakanilangizapo chisomo? ⁸ Kodi chi pangano chake chokululupilika chinayenda mwamuyaya? Kodi lonjezo yake inakangiwa mwamuyayaya? ⁹ Kodi Mulungu anaibala kunkala wachisomo? Kodi ukali wake unasiliza chifundo chake? Selah ¹⁰ Ninakamba, "Ichi ni chisoni changa: Kuchinja kwa kwanja ya manja ya Mwambamwamba kuli ise." ¹¹ Koma nizakumbukila nchito zanu Yah; nizakumbukila vodabwisa vanu vakudala. ¹² Nizaganiza nchito zanu zonse, na ku viganiza ¹³ Njila yanu, Mulungu, niyoyela; ni mulungu wabwanji angalinganize kuli Mulungu watu? ¹⁴ Ndimwe Mulungu muma chita vodabwisa; mwavumbulusa mpamvu zanu mu mitundu ya bantu. ¹⁵ Munapulumusanya bantu banu na mphanvu zanu zikulu, bobadwa mumbuyo mwa Yakobo na Yosefe. Selah ¹⁶ Manzi yanakuonani, Mulungu; manzi yanakuonani, banachita manta; kuya kunanjenjemela. ¹⁷ Makumbi inatila manzi pansi; makumbi ya nvula yanapasa liwi; mivi yanu inambululuka. ¹⁸ Liwu yanu ya mabingu inanveka mu mpepo; mphezi zinavininkila ziko; ziko inanjenjemela na kunyang'anya. ¹⁹ Njila yanu inapita munyanja na mumanzi yowinduka, koma mapazi yanu sanaoneke. ²⁰ Munasogolela bantu banu ngati nkosa na kwanja ya Mose na Aroni.

Chapter 78

¹ Nvelani kupunzisa kwanga, bantu banga, nvelani mau ya pakamwa panga. ² Nizasegula pakamwa panga mumafanizo; Nizayimba pa vintu vobisika kudala. ³ Ivi ni vintu vamene tina nvela na kupunzila, vamene makolo batu banatiuza. ⁴ Sitizavisunga kuli bana babo. Tizauza bobadwa pasogolo pali bosatila za nchito zotamandika za Yehova, mphamvu zake, na vodabwisa vamene anachita. ⁵ Chifukwa anankazikisa mapangano muli Yakobo ndipo nakuika lamulo mu Israeli. Analamulila makolo yatu kuti bazipunzisa bana babo. ⁶ Analamulila ivi kuti bobadwa posogolo ba ngazibe malamulo yake, bana bamene sibanabadwe, kuti nabeve bakaziuza bana babo. ⁷ Mwaicho bazaika chiyembekezo chabo muli Mulungu kusaibala nchito zake, koma kusunga malamulo yake. ⁸ Ndipo sibazankala monga makolo yabo mbadwo, bamene banali na ntonta na wosanvelela, wobadwa pasogolo ba mitima yabo zinali yoongoka, na mzimu yabo sunazipeleka na sibanali bokulupilika kuli Mulungu. ⁹ Bafuraimu banali na mauta, koma banabwelela kumbuyo pa siku yankondo. ¹⁰ Sibanasunge chipangano na Mulungu, banakana kumvela malamulo yake. ¹¹ Banaibala nchito zake, vodabwisa zamene anabaonesa. ¹² Banaibala vodabwisa vamene banachita pamenso pa makolo yabo mziko ya Igiputo, mziko ya Zoani. ¹³ Anagabanisa nyanja, nakubasogolela kuijumpa; anaimilika manzi monga chipupa. ¹⁴ Muzuba anabasogolela na mtambo, na kuwala kwa mulilo usiku bonse. ¹⁵ Anang'amba myala mchipululu, na ku bapasa manzi yochuluka, yokwana kuzama nyanja. ¹⁶ Analengesa misinje kuchoka mu mwala na manzi kuyyenda monga misinje. ¹⁷ Koma anapitiliza kumchimwila na kupandukila Wammwambamwamba muchipululu. ¹⁸ Banasusa Mulungu mumitima mwabo popempa chakudya kuti akutise zilakolako zabo. ¹⁹ Banakamba moshushana na Mulungu; bana kamba, "Kodi Mulungu angatiyalile tebo mucipululu?" ²⁰ Onani, pamene anakanta thantwe, manzi yana paka, na misinje inasefukila. Koma kodi angabapasenso mkate? Anga bakonzele nyama bantu bake?" ²¹ Pamene Yehova ananvela ivi anakalipa; mwaicho moto wake unayaka pa Yakobo, na ukali wake unagwela Israeli, ²² popeza sanakhulupilila Mulungu, na chipulumuso chake. ²³ Koma analamulila kutambo, Na kusegula seko za kutambo. ²⁴ Iye anabavumbisila mana kuti badye, na kubapasa tiligu yochokela kumwamba. ²⁵ Bantu banadya mkate ya bangelo. Banabatumizila chakudya chochuluka. ²⁶ Anachitisa mpepo ya kumwamba kumbululuka kumwamba, na mpamvu yake anasogolela mphepo ya kumwela. ²⁷ Anabagwesela nyama monga kalukungu, nyoni zambili monga mchenga wa kunyanja. ²⁸ Anagwa pakati pa msonkano wabo, kuzungulila mahema yabo. ²⁹ Mwaicho banadya na kukuta. Anabapasa vamene banali navo na chilaka. ³⁰ Koma; sibanazulise paneapo; chakudya chinali chikali mukamwa mwabo. ³¹ Mwaicho ukali wa Mulungu unawaukila na kubapaya wampamvu maningi pali eve. Analeta banyamata ba Israeli. ³² Chingakale ichi, banapitiliza kuchimwa na kusakulupilila zodabwisa zake. ³³ Mwaicho Mulungu anafupikisa masiku yabo; zaka zabo yanazula na manta. ³⁴ Ntawi zonse pamene Mulungu anali kubasausa, banali kuyamba kumufunafuna, na kubwelela na kumusakalisa. ³⁵ Bangakumbukile mu mutu mwabo kuti Mulungu ndiye thantwe yawo ndiponso kuti Mulungu Wamumwambamwamba ndiye anali mpulumusi wabo. ³⁶ Koma bangamunyengelela na pakamwa pabo na kubanama na mau yao. ³⁷ Pakuti mitima yao isanakazikike pa eve ndipo sibana nkale nachikulupulilo kuli chipangano lake. ³⁸ Koma eve, ponkala wachifundo, anakululukila mpulupulu zao, na kukusabaononga. Ehe, ntawi zambii anabweza ukali wake, ndipo sanause naukali wake onse. ³⁹ Anakumbukila kuti banapangiwa tupi, mpepo yamene imapita na kusabwelela. ⁴⁰ Kabilikabili pamene bagnamupandukile muchipululu na kumumvesa chisoni mumadela ouma! ⁴¹ Mobwelezabweleza anasusa Mulungu na kukumukudwisa Woyela wa Israeli. ⁴² Beve sanaganizepo za mpamvu zake, mwamene anabapulumusila mumanja mwa badani, ⁴³ pamene anachita zozizbisa zake ku Iguputo na zodabwisa zake muchigao cha Zoani. ⁴⁴ Anabwelela misinje ya Iguputo kunkala magari kuti asamwe mumisinje yao. ⁴⁵ Anatumiza tizilombo zainzi zamene zina badya, na bachule bamene banaononga ziko yao. ⁴⁶ Anapeleka zokolola zawo kwa ziwala, na ntchito yao kuli dzombe. ⁴⁷ Anaononga mipesa yao na matalala na mikuyu yao na matalala yambili. ⁴⁸ Anagwesa matalala pa ng'ombe zawo na mphezi pa zibeto zawo. ⁴⁹ Ukali wa mkwiyo wake unabagwela. Anatumiza ukali, ukali, na zobaba, monga ntumwi za kuononga; ⁵⁰ Anakonzela mkwiyo wake njila; sanabapulumuse ku infa, koma anawapeleka ku mlili. ⁵¹ Anapaya bana boyamba mu Iguputo, oyamba ba mpamvu zao mumahema ya Hamu. ⁵² Anasogolela bantu bake monga nkosa, anabasogolela muchipululu monga gulu ya nkosa. ⁵³ Anabasogolela moteteza na kulibe manta, koma nyanja inamiza badani babo. ⁵⁴ Mwaicho anabapitisa ku malile ya ziko yake yopatulika, kupili yamene kwanja yake yamanja inapeza. ⁵⁵ Anapilikisha bamitundu pamenso pabo ndipo anapasa choloba chabo. Anankazika mitundu ya Israeli mumahema yabo. ⁵⁶ Koma banasusa na nakumupandukila Mulungu Wamumwambamwamba, na kusasunga malamulo yake. ⁵⁷ Banali osakulupilika na kuchita zachinyengo monga makolo yabo; banali osadalilika monga uta wolakwika. ⁵⁸ Mwaicho anamukalipisa na malo yabo yokwezeka, na kumukwiyisa na kakaliyo kaukali na tumulungu twabo. ⁵⁹ Pamene Mulungu ananvela ivi, anakalipa maningi anakankanilatu Asraeli. ⁶⁰ Anasiya malo opatulika yaku Silo, + chihema chamene

bankakala pakati pa antu. ⁶¹ Anavomeleza mpamvu zake kugwiliwa, nakupeleka ulemelelo wake mumanja ya badani. ⁶² Anapeleka bantu bake kuli lupanga na kubakwiyila cholowa chake. ⁶³ Moto unanyekesa banyamata babo, na basikana babo banalibe nyimbo zaukwati. ⁶⁴ Bansembe babo banagwa na lupanga, na bakazi babo wofelewa sanalile. ⁶⁵ Yehova anagalamuka monga muntu wa mutulo, monga wankondo wopunda chifukwa cha vinyo. ⁶⁶ Anabweza badani bake; anachitisa manyazi yosasila. ⁶⁷ Anakana chihema cha Yosefe, ndipo sanasanke chitundu cha Efuraimu. ⁶⁸ Anasanka ya Yuda na pili ya Zioni yamene analikonda. ⁶⁹ Anamanga malo yake yopatulika monga kumwamba, ngati ziko yamene anankazikisa wamuyayaya. ⁷⁰ Anasanka Davide, mutumiki wake, anamtenga mukola ya nkosa. ⁷¹ Anamutenga posatila nkosa na bana babo, kuyenda naye kuti mubusa wa Yakobo, bantu bake, choloba chake cha Israeli. ⁷² Davide anawaweta na mtima osagawanika, na kuabasogolela na luso ya manja ake.

Chapter 88

Nyimbo, salimo ya bana bamuna ba Kora; ku oyimba mukulu; yopangiwa musitailo yaku Mahalati Leanoti. Nyimbo ya Hemani Mwezra. ¹ Yehova, Mulungu wa chipulumuso changa, nilila muzuba na usiku pameso panu. ² Mvelani pempelo yanga; mvelani kulila kwanga. ³ Chifukwa nazuliwa na mavuto, na moyo wanga wafika kumanda. ⁴ Banthu banichita kwatii muntu oyenda kumugodi; Ndine muntu alibe mphamvu. ⁵ Nadasiyiwa pa bakufa; Nili ngati bakufa bamene bali kumanda, bamene simusamalila chifukwa bachosewa mu mphamvu yanu. ⁶ Mwaniika pansu mungodi, mumalo ndi yakuya. ⁷ Ukali wanu wanilemela ine, na mphamvu yapempo yanu yanigwesa; Selah ⁸ Chifukwa cha imwe, banzanga bamanitaba. Mwanipanga chadabwisa mumenso yao. Nazungulukiwa ndipo siningatabe. ⁹ Menso yanga yalema na mavuto; Siku yonse nililila kuli imwe, Yehova; Natambasulila manja yanga kuli imwe. ¹⁰ Kodi muzachita zodabwisa kubakufa? Kodi bakufa bazauka nakutamandani? Selah ¹¹ Kodi chipangano chakukulupilika kwanu kambiwa mumanda, cikhulupiro canu kumanda? ¹² Kodi vodabwisa vanu vizazibika mumdima, kapena chilungamo chanu mumalo mowala? ¹³ Koma inizalila kuli imwe, Yehova; mumawa pempelo yanga imabwela pameso panu. ¹⁴ Yehova, niciani munikana? Nichiani mubisa nkhope yanu? ¹⁵ Nakhala ovutisiyiwa ndipo pafupi nakufa kuyambila kuufana wanga. Navutika kuboyofya banu; Nataya mtima. ¹⁶ Vochitika vanu voyofya vapita pali ine, ndipo voyofya vanu vocitika vani ononga ine. ¹⁷ Vanizunguluka ngati manzi siku onse; Onse bananizunguluka. ¹⁸ Mwanichosela banzanga na oniziba kuli ine. Choniziba chabe apa ni mumdima.

Chapter 89

Nyimbo ya Etani waku Ezara. ¹ Nizayimba zavocitika va chipangano chachikulupililo cha Yehova muyayaya. Nizakamba zachilungamo cha chabo badwa musogolo. ² Chifukwa nakamba, "Chipangano cha chikhulupililo chakhazikika muyayaya; kukulupilila kwanu kwakhazikisika kumwamba. ³ Napangana chipangano na osankiwa banga, ndalumbila kuli Davide wanchito wanga. ⁴ Nizakhazikisa bobadwa mumbuyo bako muyayaya, ndipo nizakhazikisa ufumu wako ku obandwa musogolo." Sela ⁵ Kumwamba kutokoza vodabwisa vanu, Yehova; chilungamo chanu chitokozewa musonkhano wa oyela. ⁶ Pakuti nindani mumakumbi wamene angalinga naimwe Yehova? Nindani pabana bamuna bamilungu wamene ali ngati Yehova? ⁷ Ni Mulungu olemkezeke kwambili musonkhano wao yela ndipo niwabwino kuli bonse bomuzunguluka. ⁸ Yehova Mulungu wa makamu, alina amphamvu ngati Imwe Yehova ndani? Chilungamo chanu chikuzungulukani. ⁹ Imwe mulamulila nyanja yoyofya; mafunde yakabwela, mumayazizilika. ¹⁰ Munaphwanya Rahabi ngati muntu wakufa. Munatabisa badani banu n kwanja yanu yamphumvu. ¹¹ Kumwamba ni kwanu, na ziko yapasi. Imwe mupanga ziko yapasi na vonse vilimo. ¹² Munalenga kumpoto na kumwela. Tabori na Hermoni bakondwela muzina yanu; ¹³ Muli na gulu yamphamvu na kwanja yamphamvu, ndipo kwanja yanu yamanja niitali. ¹⁴ Chilungamo na kuweluzi ndiye maziko ya mupando wanu. Chikondi na kukulupilika kosasila kumabwela pameso panu pamaso panu. ¹⁵ Nibodaliska bantu bamene bakuyamikani! Yehova, bayenda mukuyela pameso panu; ¹⁶ Bakodwela muzina yamukondwela muzina yanu siku yonse, na m'chilungamo chanu bakukwezani. ¹⁷ Ndimwe bamphamvu zikulu, ndipo mu chisomo chanu ndise bopambana. ¹⁸ Pakuti chikopa chathu ni chanu Yehova; mfumu yathu ni ya oyela wa Isiraeli. ¹⁹ Kalekale munakamba m' masomphenya yabokhulupirika banu; munakamba, "Naika kolona pali wamphamvu. Naimya bosankiwa pa bantu. ²⁰ Nasakha Davide mtumiki wanga; Na mafuta yanga yoyela kumuzoza. ²¹ Kwanja yanga izamugwila; kwanja yanga uzamukosesa. ²² Palibe mudani wamene azamunama; palibe mwana mwamuna oipa wamene azamudyakilila. ²³ Nizaphwanya badani bake pameso pake; Nizapaya bamene sibamukonda. ²⁴ Muchilungamo changa na chipangano chakukulupilika kwanga kuzangala naye; muzina yanga eve azapambana. ²⁵ Nizaika kwanja yake panyanja, na kwanja yake yamanja pa mitsinje. ²⁶ Eve azaitana kuli ine, 'Imwe ndimwe batate banga, Mulungu wanga, ndipo nimwe mwala wa chipulumutso changa. ²⁷ Nizamuka kukhala mwana muna oyamba wanga, okwezekewa manigi pa mafumu ya ziko yapansi. ²⁸ Nizaikilako chipangano chakukulupilika changa mwamuyayaya; ndipo chipangano changa chizakhala na eve. ²⁹ Nizapanga bobadwa mumbuyo mwake kupilila muyayaya, na mpando wa ufumu wake kukhale monga thambo makumbi. ³⁰ Ngati bana bake basiya lamulo yanga ndipo sibayanda mumalemba yanga, ³¹ Ngati baphwanya malamulo yanga na kusunga malamulo banga, ³² pamene apo nizabalanga na ndodo ndipo machimo yao namukwingwilima. ³³ Koma sinizachosa chikondi changa pali eve kapena kusakulupilika kwake pa lonjezo yanga. ³⁴ Sinizaphwanya chipangano yanga, kapena kusingha mau ya milomo yanga. ³⁵ Nalumbila pakuyela kwanga — sinizanama kuli Davide: ³⁶ bobadwa mbuyo bake bazakhala muyayaya, ndipo ufumu wake uzakhalapo pameso panga muzuba. ³⁷ Nizaika muyayaya ngati mwezi, khulupilika m'mwamba." Sela ³⁸ Koma imwe simufuna ndipo mwakana; mwakalipila mfumu yozozewa. ³⁹ Mwataya chipangano yawa nchito wanu. Mwaipisa chisote cha ufumu pansi. ⁴⁰ Mwangwesa chiumba chake onse. Mwaononga malo yolimba yake. ⁴¹ Bonse bamene bapita bamubela. Akhala chintu chonyasa ku banzake bake. ⁴² Mwakweza kwanja yamanja ya badani bake; mwakondwelesa badani bake bonse. ⁴³ Mwapindamula lupanga yake yakutwa, ndipo simunatenge kunkhondo. ⁴⁴ Mwabwelesa ulemelelo wake; mwagwesa pansi mpando wa ufumu wake. ⁴⁵ Mwafupikisa masiku ya ufuna wake; Mwamuvesa soni. Selah ⁴⁶ Kufika liti, Yehova? Kodi muzazibisa muyayaya? Kodi ukali wanu uzayaka ngati mulilo kufikila liti? ⁴⁷ Ganizaniponi pa ufupi wa nthawi yanga, ndi kodi munapanga balibe nchito bonse bana babantu! ⁴⁸ Ndani angakhale na moyo wosafa, kapena kupulumusa moyo wake ku kwaanja ya Manda? Selah ⁴⁹ Mbuye, vochitika vanu va chipangano cha kukulupilika kwanu chamene munalapila pali Davide mukukulupilika kwanu kuli kuti? ⁵⁰ Kumbukilani, Yehova, kunyozewa kwame wanchito wanu, ndipo mumtima mwanga muli manyozo yamitundu; ⁵¹ Badani banu bachitila mwano, Yehova; batukana mayendedwe yao ozozewa banu. ⁵² Olemkezeke Yehova muyayaya. Amene Amene.

Chapter 90

Pemphelo ya Mose muntu wa Mulungu. ¹ Yehova, mwakhala kopothabila mumibado yonse ² Malupili yakalibe kupangiwa, kapena mukalibe kupanga ziko yapansi na ziko yapansi, kuyamba nthawi yosasila kufikila nthawi yosasila, imwe ndimwe Mulungu. ³ Mubweza muntu ku doti, ndipo mukamba, “Bwelelani, imwe bobadwa mumboyo bantu; ⁴ Pakuti zaka masazandi pameso panu yali ngati sikuyapita, ngati ulonda wa usiku. ⁵ Mubapyanga monga ni chigumula,ndipo bagona; mumawa bazakhala ngati msipu ophuka. ⁶ Mumawa vizashuma na kukula; mazulo viza mafota, naku yuma. ⁷ Muchilungamo, tadyewa na ukali wanu, ndipo kukalipa kwanu kati yofya. ⁸ Mwaika machimo yathu pameso panu, machimo yathu yobisika mulaiti ya nkhope yanu. ⁹ Moyo wathu wapita pansu pa ukali wanu; zaka zathu ziyenda musanga ngati kufuza. ¹⁰ Vaka Vathu vili 70, kapena 80, ngatili namoyo wabwino; koma ngakhale vaka vathu vabwino manigi vimakhala na mavuto nz chisoni. Inde, yamapita musanga, ndipo ise timambuluka. ¹¹ Ndani aziba kukula kwa ukali wanu, na kukalipa kwanu kulingana na kuyopa imwe? ¹² Choncho tiphunziseni kuganizila moyo wantu kuti tikhale na moyo wanzelu. ¹³ Bwelelani, Yehova; Izatenga nthawi itali bwanji? Chitilani chifundo banchito banu. ¹⁴ Tibveseni bwino mumawa na chipangano chanu chakukhulupilika kuti tikondwele na kukondwela masiku yantu yonse. ¹⁵ Tikondweleseni monga muma siku munatisausa, na zaka zamene tinavutika nazo. ¹⁶ Lekani banchito banu baona ntchito yanu, na baona bantu baone ulemelelo wanu. ¹⁷ Lekani ubwino wa Mbuye Mulungu wantu; inde, chulukisani nchito yamanja yantu.

Chapter 91

¹ Eve wamene akhala mumalo yamumwamba azakhala mu chinwili nvili cha mphamvuzonse. ² Nizakamba pali Yehova, "Eve nikotabila kwanga na malo yabwino yanga, Mulungu wanga, wamene nimkhulupilila. ³ Pakuti eve azakupulumusani ku msampha wa ogwila nyama na kumlili opaya. ⁴ Eve bisani na mapapiko yake, ndipo pansipa mapiko yake uzapeza pothabila. Kukulupilika kwake na chishango ni vachitetezo. ⁵ Siuzayopa voyofya usiku, kapena mivi yombuluka mumazulo, ⁶ kapena mulili oyenda mumdima, kapena chiwonongeko chowononga mumazulo. ⁷ Banthu 1,000 bangagwe pambali pako, nabenangu 10,000 kukwanja yako yamanja, koma sibazafika kuli iwe. ⁸ Uzoona chabe na chilango cha boipa. ⁹ Pakuti Yehova ndiye kotabila kwanga! Mupange wakumwamba kotabila kwako. ¹⁰ Palibe choipa chizakupezani; vovutisa siviza bwela pafupi nanyumba yako. ¹¹ Pakuti tuma bangelo bake kuti bakuchingileze, bakulondeni munjila yanu yonse. ¹² Bazakunyamula na kwanja yako kuti menye kwendo yako pamwala. ¹³ Udzaphwanya mikango na mbawala pansipamendo yako; udzapondaponda mikango ya mikango na njoka. ¹⁴ Chifukwa chakuti niwoziipeleka kuli ine, nizampulumusa. Nizamuchingiliza chifukwa ni okhulupilika kuli ine. ¹⁵ Akaniitana, nizamuyankha. Nizakhala naye mumabvuto; Nizamupasa kupamabana ndipo nizamulemekeza. ¹⁶ Nizamuvesa bwino na utali wa masiku yake, na kumuonesachipulumuso changa.

Chapter 92

Salimo, nyimbo ya siku ya Sabata. ¹ Ni chintu chabwino kuthokoza Yehova, na kuyimba zotamanda zina yanu, waku mwamba, ² kulengeza chipangano chanu mumamawa, ndi chilungamo chanu usiku ulionse, ³ na chitolilo cha zingwe zili 10, na nyimbo ya zeze. ⁴ Pakuti imwe, Yehova mwanivesa bwino chifukwa cha vochita vanu. Nizayimba mokondwela chifukwa cha vocita va manja yanu. ⁵ Ntchito yanu ni yaikulu, Yehova! Maganizo yanu ni yozama kwambili. ⁶ Opusa saziba, kapena wopusa sazindikila ivi: ⁷ Pamene oipa amela ngati uzu, ndipo ngakhale ochita voipa bonse bamapaka, bazawonongewa kosatha. ⁸ Koma imwe, Yehova, muzakhala mukulamulalila muyayaya. ⁹ Onani badani banu, Yehova! Inde, Onani badani banu. Beve bazaonongeka! Bonse bamene bamachita voipa bazatabisiwa. ¹⁰ Mwanyamula nyanga yanga ngati nyanga ya ng'ombe; Nazozewa na mafuta yasopano. ¹¹ Meso yanga yaona kugwa kwa badani banga; matu yanga yanamvela za kuonongeka kwa badani banga boipa. ¹² Olungama bakula bwino ngati mgwalangwa; bakula bwino ngati mkungudza wa ku Lebano. ¹³ Beve nibo shangiwa munyumba ya Yehova; Beve bakula bwino mulo ya Mulungu wathu. ¹⁴ Bamabala vipaso olo kuti bakula; beve bamakhala owoneka bwina na obilibila, ¹⁵ bazakamba kuti Yehova ni olungama. Eve ndiye mwala wanga, ndipo muli eve mulibe osalungama.

Chapter 93

¹ Yehova alamulila; abvala ulemelelo; Yehova azibvalika nakuzibisa na mphamvu. Ziko yankazikisiwa; siinga vendezewe

² Mpando wanu wa ufumu wakhazikika kuyambila kalekale; ndimwe koyambilila nthawi zosayamba. ³ Nyanja nyamuka, Yehova; akweza mau yao; mafunde ya munyanja yapwanya nakupunda. ⁴ Pamwamba pa kupwanya mafunde yambili, mafunde yamphamvu ya munyanja, Yehova wa mumwamba ndiye niwamphamvu. ⁵ Malamulo yanu ni odalilika manigi; kuyela kwanu kuwamisa nyumba yanu, Yehova, masiku yanu yambili;

Chapter 94

¹ Yehova, Mulungu amabwezela chilango, Mulungu wobwezela chilango, wawala pali ise. ² Nyamukani, woweluza ziko yapansi, pelekani ku ozivela kuyenela navo. ³ Kodi boipa bazasangalala mpaka liti, Yehova? ⁴ Bachosa mau yao ozitukumula; bonse bochita voipa azinvela. ⁵ Baphwanya bantu banu, Yehova; bavutisa mtundu ya bantu banu. ⁶ Bapaya mukazi wamasiye na mlendo okhala muziko yawo, nakupaya bana balibe batate. ⁷ Bakamba, "Yehova saona, Mulungu wa Yakobo sadziba." ⁸ Muvesesa, bantu opusa imwe! Opusa imwe, mudzaphunzila liti? ⁹ Eye wamene anapanga matu, samavela kodi? Eve wamene anapanga menso, saona? ¹⁰ Eve wamene amalanga mitundu, kodi salanga? Eve wamene amapasa muntu nzelu. ¹¹ Yehova amaziba maganizo ya bantu, ali nthunzi. ¹² Odala muntu wamene mumalangiza, Yehova, bamene mumphunzisa mulamulo yanu. ¹³ Mumampasa kupumula mumasiku ya mavuto, mpaka chisengu choipa ikumbiwa. ¹⁴ Pakuti Yehova sazasiya bantu bake kapena kusiya choloba chake. ¹⁵ Pakuti kuweluzwa khuzalako chabolungama; ndipo bonse bolungama mtima bazakonka. ¹⁶ Ndani azani pulumusa kubochita voipa? Nindani azanitandiza mumalo mwanga ku boipa? ¹⁷ Yehova nga ananitandiza, Nganina gona panso pamalo yazi. ¹⁸ Pamene ninakamba, "Mendo yanga yatelemuka," Chipangano chikhulupililo chanu, Yehova, ananigwilila. ¹⁹ Pamene anisamalila muli ine muli bambili, zotonthoza zanu zimanikodwelesa. ²⁰ Kodi mpando wa ufumu ugwilizane na chiwonongeko muli imwe, wamene apanga malamulo osalungama? ²¹ Beve bamapangana voipa kuti bapayeaphe bolungama na kuweluzwa muntu wosalakwa kupaiwa. ²² Koma Yehova ndiye nyumba itali yanga, na Mulungu wanga ndiye mwala otabilko wanga. ²³ Eve azabwelesa machimo yawo ndipo azabaononga chifukwa cha kuipa kwao. Yehova Mulungu wathu azabajuba.

Chapter 95

¹ Bwelani, tiyimbile Yehova; tiyeni tiyimbe mokodwela kumwala wa chipulumuso chantu mokondwela. ² Tiyeni tingene pameso pake ndi kupembeza; tiyeni timumbile eve masalimo yo thokoza. ³ Pakuti Yehova ni Mulungu wamukulu na Mfumu ikulu kuchila milungu yonse. ⁴ Mumanja yake muli vozama va ziko yapansi; kotalimpa kwama lupili nikwake. ⁵ Nyanja ni zake, chifukwa anaipanga, ndipo manja yake ynapanga malo. ⁶ Bwelani, timupembeze na gwanda pansi; tiyeni tigwade pamaso pa Yehova, opanga wathu: ⁷ Pakuti eve ni Mulungu wathu, ndipo ise ndise bantu ba pabusa pake, ndi nkhusa za mumanja yake. Lelo, kuti mumvele mau yake! ⁸ “Musakosese mtima wanu, monga pa Meriba, kapena pa siku ya Masa muchipululu, ⁹ pamene makolo yanu yananiyesa na kuniyesa, olo kuti banona nchito yanga. ¹⁰ Mu zaka 40 neze okalipa na mibado uja, ndipo ninakamba, 'Aba ni bantu bamene mitima yao yasoba; sibaziba njila zanga.' ¹¹ Nichifukwa chake ninalumbila mukukalipa kwanga, kuti sibazaloba mu opulilako yanga.

Chapter 96

¹ Oh, imbilani Yehova nyimbo yamanje; imbilani Yehova, ziko yonse yapansi. ² Imbilani Yehova, lemekezani zina yake; pundani chipulumuso chake siku na siku. ³ Kambani ulemelelo wake mumitundu, vodabwisa vake ku mitundu yonse. ⁴ Pakuti Yehova ni mukulu ndipo ayenela kulemekeza kwambili. Ayenela kuyopa kuposa milungu ina yonse. ⁵ Pakuti milungu yonse ya mitundu ni mafano, koma ni Yehova wamene analenga kumwamba. ⁶ Ulemelelo na ukulu vili pamenso pake. Mphamvu naku kukongola vili mumalo yake yopatulika. ⁷ Pelekani kuli Yehova, imwe mafuko ya bantu, lemekezani Yehova chifukwa cha ulemelelo wake na mphamvu zake. ⁸ Pasani Yehova ulemelelo oyenela. Bwelesani chopeleka na kubwela mubwalo yake. ⁹ Gwadani kuli Yehova mu ulemelelo wa chiyelo; njenjemela pamenso pake, ziko yapansi yonse. ¹⁰ Kambani pakati pa mitundu, "Yehova alamulila." Ziko yapansi inkazikika; singanyang'anyisiwe. Amaweluza mwachilungamo mitundu ya bantu. ¹¹ Lekani kumwamba kukondwele, na ziko yapansi ikondwele; nyanja iwulume na vonse vili mwamene vipunde mokondwela. ¹² Minda ikondwele na vonse vili mwamene. Ndipo mitengo yonse yamunsanga ipunde mokondwela. ¹³ pamenso pa Yehova, chifukwa abwela. Abwela kuweluza ziko yapansi. Azaweluza ziko yapansi na chilungamo ndipo mitundu ya bantu na kukulupilika kwake.

Chapter 97

¹ Yehova alamulila; lekani ziko yapansi ikondwele; visumbu vambili vikondwele. ² Makumbi na mudima vimuzunguluka. Kululungama na chiweluzo chabwino ndiye maziko ya mupando wake wachifumu. ³ Mulilo upita pasogolo pake na kunyekesa badani bake pambali ponse. ⁴ mphezi zake ziunikila ziko yapansi; ziko yapansi iona nakunjenjema. ⁵ Mapili yasungunuka monga sela pamenso pa Yehova, Ambuye wa ziko yonse yapansi. ⁶ Mulengalenga ukambilila chilungamo chake, ndipo mitundu yonse yaona ulemelelo wake. ⁷ Bonse balambila mafano yosema bazachita manyazi, bamene bazitamandila ma mafano yalibe kantu- bamugwadila eve, milungu yonse! ⁸ Ziyoni ananvela nakukondwela, ndipo minzi ya Yuda inakondwela chifukwa cha malemba yanu yolungama, Yehova. ⁹ Pakuti imwe, Yehova, ndimwe wamumwambamwamba pa ziko yonse yapansi. Mwakwezekewa kupita milungu yonse. ¹⁰ Imwe bamene mukonda Yehova, nakuzonda voipa! Amateteza moyo ya bokulupilika, ndipo amabachosa mumanja ya boipa. ¹¹ Kuunika kumafesedwa kuli bolungama na chisangalalo kuli bamene ba mitima yazona. ¹² Kondwelani muli Yehova, bolungama imwe; ndipo tokozani pamene mukumbukila chiyelo chake.

Chapter 98

Salimo. ¹ O, Imbilani Yehova nyimbo yamanje, pakuti acita vodabwisa; kwanja yake yamanja na kwanja yake yopatulika yamupasa chipulumuso. ² Yehova wazibisa chipulumuso chake; alangiza chilungamo chake ku mitundu yonse. ³ Akumbukila chikondi chake na kukulupilika kwa nyumba ya Israeli; malekezelo yonse ya ziko yapansi yazaona chipulumuso cha Mulungu watu. ⁴ Pundani kuli Yehova mokondwela, ziko yonse yapansi; pundani mokondwela, imbani nachisangalalo, na nyimbo zotamanda Mulungu. ⁵ Imbilani Yehova volemekeza na zeze, na zeze na nyimbo zabwino. ⁶ Na malipenga na kulila kwa lupenga, pangani chongo mokondwela pamenso ya Mfumu, Yehova. ⁷ Lekani nyanja ipunde na vonse vili mwamene, ziko yapansi na vamene vonkalamo. ⁸ Misinje itote na manja, na mapili yapunde mokondwela. ⁹ Yehova abwela kuweluza ziko yapansi; azaweluza ziko yapansi na chilungamo, na mitundu mwachilungamo.

Chapter 99

¹ Yehova alamulila; lekani mitundu injenjeme. Ankala pamwamba pa makerubi; ziko igwedezeka. ² Yehova ni mukulu mu Ziyoni; ndiye niokwezekewa pamwamba pa mitundu yonse. ³ Balemekeze zina yanu ikulu na yabwino; eve ni oyela. ⁴ Mfumu niwa yampamvu, ndipo amakonda chilungamo. Mwakazikisa chilungamo; mwachita chilungamo na chiweluzo muli Yakobo. ⁵ Tamandani Yehova Mulungu watu ndipo lambilani pa chopondapo mapazi yake. eve ni oyela. ⁶ Mose na Aroni pamozi na bansembe bake, ndipo Samueli anali pamozi na bantu banaitana zina yake. Beve banaitana kuli Yehova, ndipo anabayanka. ⁷ Anakamba nabeve kuchokela mumakumbi yoima monga chipilala. Banasunga malamulo yake na malemba yamene anabapasa. ⁸ Munabayanka, Yehova Mulungu watu. Mulungu okululuka unali kuli beve, koma wamene anabalanga volakwa vabo. ⁹ Tamandani Yehova mulungu watu, ndipo lambilani pa phili yake yopatulika, pakuti Yehova Mulungu watu ni oyela.

Proverbs

Chapter 6

¹ Mwana wanga, ngati wapeleka ndalama cha ngongole ya munzako wako wapafupi, ngati unamukongolesa munthu wamene suziba, ² wazitchela msampha na lonjezano yako, ndipo wagwiliwa na mau ya pakamwa pako. ³ Ukagwiliwa na mau yako, mwana wanga, chita ici uzipulumuse weka, popeza wagwa mukwanja ya munzako wako wapafupi; yenda ukazichepese, mukambisane milandu yako na munzako wako wapafupi. ⁴ Usagone tulo na manso yako na zikope zako sizakusile. ⁵ Zipulumuse weka ngati mbalame mukwanja ya mlenje, monga nyoni mukwanja ya msodzi. ⁶ Yangana nyelele, walesi iwe, punzila njila zake, unkhale wanzelu. ⁷ Ilibe musogoleli, mukulu, kapena wolamulila, ⁸ koma ikonza zakudya zake mumalimwe nakusunga zamene izadya mu nthawi yokolola. ⁹ Ugoni mpaka liti, walesi iwe? Muzauka liti mutulo yanu? ¹⁰ "Kugona pangono, kukusila pangono, kupeteka manja pangono kuti mupumule" - ¹¹ ndipo umphawi wanu uzabwela monga wachifwamba na zosowa zanu ngati musilikali wonkhala na zida. ¹² Munthu wachabechabe - munthu woyipa - ankhala na mau okhotakhota, ¹³ akuzidinizila na manso yake, akuloza na jala zake. ¹⁴ Amakonza zoyipa na chinyengo mumtima mwake; nthawi zonse amayambisa mikangano. ¹⁵ Chifukwa cake soka yake izamugwela mukanthawi kochepe; mukamphindi azasweka kosachilisiwa. ¹⁶ Pali vinthu visanu na imodzi vamene Yehova amazonda, zisanu na ziwili zonyansa kwa eve: ¹⁷ Manso ya munthu wozitukumula, lilime yonama, manja okhesa mwazi ya banthu ya wosacimwa, ¹⁸ mutima wokonza ziwembu zoyipa, mendo yothamangila kucita zoyipa, ¹⁹ mboni yolankhula maboza na woshanga mikangano pakati pa abale. ²⁰ Mwana wanga, mvela lamulo ya batate bako osasiya chiphunziso cha amai bako. ²¹ Yamange pamutima nthawi zonse; uyamange pamukosi pako. ²² Pamene muyenda, vizakusogolelani; pamene mwagona pansu, azakuyanganila; ndipo mukauuka, yeve yazakuphunzisani. ²³ Pakuti malamulo ni nyali, na chiphunziso ichi ni nyali; chilangizo camene chimabwela ni njila ya umoyo. ²⁴ Ima kuchingiliza ku mukazi wachiwelewele, Kumau yotelela ya mukazi wachiwelewele. ²⁵ Usasilile kukongola kwake mumtima mwako ndipo asakukole na nsili zake. ²⁶ Kugona na hule kungawononge mutengo wa buledi, koma mukazi wa wina angawononge umoyo wako. ²⁷ Kodi munthu anganyamule moto pachifuba pake kosashoka zovala zake? ²⁸ Kodi munthu angayende pa makala yamoto osapya mu mendo mwake? ²⁹ Ndiye mwamene munthu woloba kwa mukazi wa muzake wake wa pafupi; wamene akukhuza sazaleka kulangiwa. ³⁰ Banthu musanyoza wakuba ngati aba kuti apeze chakudya ali na njala. ³¹ Koma akagwiliwa, azibwezela kasanu na kawili zamene anaba; ayenela kusiya chilichonse chamutengo wapatali chili munyumba mwake. ³² Wochita chigololo alibe nzelu; wochita zamene izi aziwononga eka. ³³ Vilonda na manyazi nizomuyenela ndipo manyazi yake sazafufutiwa. ³⁴ Pakuti nsanje ikwiya munthu; sazachitila chifundo pobwezela chilango. ³⁵ Sazalandila malipilo ndipo sangaguliwe, ngankhale mumupase mphaso zambili.

Chapter 7

¹ Mwana wanga, sunga mau yanga na kusunga malamulo yanga mukati mwako. ² Sunga malamulo yanga unkhale na umoyo, ndipo usunge malangizo yanga monga apulosi mu linso yako. ³ Uvimange pa vimbombo vako; zilembe pa cholembapo cha mutima wako. ⁴ Nena kwa nzelu, "Iwe ndiwe mulongo wanga," itani kuvesesa mbale wako, ⁵ kuti uziteteze kwa mukazi wachigololo, kuchokela kuli mukazi wachiwelewele amene amapanga mau yotelela yake. ⁶ Pa zenela ya nyumba yanga ninayangana pa latisi. ⁷ Ninayangana banthu wosachangamuka, ndipo ninaona kuti pakati pa ba anyamata panali wachinyamata wopanda nzelu. ⁸ Munyamata uyu anapita mumusewu pafupi na mphambano ya mayiyo, nikupita kunyumba kwa mukazi uyu. ⁹ Kunali mumazulo, mazulo ya usana, nthawi ya usiku na mudima. ¹⁰ Kwamene mukazi wina anakumana na eve, anavala ngati hule, na mutima waboza. ¹¹ Banali waphokoso na wosokela; mendo yake sanankhale kunyumba. ¹² Manje mumisewu, na mumisika, na pobisalila pa ngodya zonse. ¹³ Ndipo anamugwila na mphamvu, naku mupsompsona, nkhope yake yamphamvu anamuuza eve kuti, ¹⁴ Napeleka lelo nsembe yamutendele, nachita zowinda zanga, ¹⁵ manje nabwela kukumana na iwe, kufunafuna nkhope yako, ndipo ine nakupeza. ¹⁶ Nayanzika zofunda pa bedi panga, nsalu zamitundumitundu za ku Igupto. ¹⁷ Ndawaza pabedi yanga mure, aloe, na sinamoni. ¹⁸ Tiyeni, tikhute na chikondi kufikila mumawa; tiyeni tisangalale na nchito zachikondi. ¹⁹ Pakuti mwamuna wanga palibe kunyumba kwake; ayenda ulendo wautali. ²⁰ Anatenga thumba ya ndalama pamozi naye; azabwela pa siku ya mwezi wathunthu." ²¹ Na kulankhula zambili anamutembenuza; na milomo yake yosalala anamsokereso. ²² Mwazizizi anayenda kuli eve monga ng'ombe yopita kukapayiwa, ndipo ngati chipuba chalangiwa na maunyolo ²³ mpaka muvi ulasa pachiwindi chake. Anali monga nyoni yothamangila mumsampha. Sanazibe kuti zikanamutayisa moyo. ²⁴ Manje, bana banga, mvelani kuli ine; tcherani khutu ku mawu a pakamwa panga. ²⁵ Mutima wako usapatukile kumayendedwe yake; musasocheresewe mumayendedwe yake. ²⁶ Wagwesa banthu bambili olasiwa; bamene eve anapaya ni bambili. ²⁷ Nyumba yake ili munjila za kumanda; amasikira ku zipinda zamumudima za infa.

Chapter 18

¹ Muntu wamene amazipatula amasakila sakila vofuna vake ndipo amalimbana na nzelu zonse. ² Chofunta sichikondwela na kumvesesa, koma kuwulula va mumutima mwake. ³ Woipa akabwela, manyozo yamabwela pamozi na manyazi na manyozo. ⁴ Mau ya mukamwa mwa muntu ndiye manzi yozama; Kasupe wa nzelu ndiye mumana wokunkuluka. ⁵ Kukondela woyipa sikwabwino, kapena kulesa wolungama mtima. ⁶ Milomo ya wofunta imaleta kukangana ndipo pakamwa pake paitana kumenyewa. ⁷ Mukamwa mwa wofunta ni chiwonongeko chake ndipo eve amaziteya musampa eka na milomo yake. ⁸ Mau ya watonzyo yali monga chakudya chabwino ndipo chimaselukila mukati mwa tupi. ⁹ Koma futi, muntu waulesi pa nchito yake ni mubale wa wamene amawononga maningi. ¹⁰ zina ya Yehova ndiye chochingiliza cholimba; wolungama atamangilamo nakupulumuka. ¹¹ Chuma cha wolemela ndiye muzinda wake utali ndipo mukuganiza kwake aona monga nichipupa chitali. ¹² Muntu akalibe kugwa mutima wake umazimvela, koma kuzichepesa kumasogolea ulemu. ¹³ Wamene amayanka akalibe kumvela ni kupusa kwake na namanyazi. ¹⁴ Moyo wa muntu uzapulumuka matenda, koma nindani angakwanise kunyamula muzimu wotaika? ¹⁵ Mtima wa muntu ochenjela umapeza nzelu ndipo matu ya wanzelu yamasakila. ¹⁶ Mpaso ya muntu ingasegule njila na kumupeleka kuli muntu wofunika. ¹⁷ Woyambilila kumupasa mulandu aoneka kuti ni wokonkakonka mpaka woshushana naye abwele nakumufunsa. ¹⁸ Mayele yamasiliza mikangano ndipo yamalekanisa boshusha bampamvu. ¹⁹ Mubale wokumudwisiwa achila muzinda wolimba, na ndeo ili monga nsimbi za linga. ²⁰ Mimba ya muntu imakuta na vipaso va mukamwa mwake; eve amakuta na vipaso va milomo yake. ²¹ Imfa na moyo vimayendesewa na lulimi, ndipo beve bamene bamakonda lulimi bazadya vipaso zake. ²² Wamene apeza mukazi apeza chintu chabwino, ndipo Yehova amamukomela mutima. ²³ Wosauka amachita kupapatila chifundo, koma wolemela amayanka mwaukali. ²⁴ Muntu wamene afuna banzake bambili aonongeka nao; Koma kuli munzake wamene amabwela pa fupi monga mubale.

Chapter 19

¹ Wosauka wamene ayenda mu ungwiwo achila muntu wo kamba mopotoloza ni wopusa. ² futi, sichabwino kunkala na chilakolako chilibe kuziba ndipo wamene amatamanga maningi amataya njila. ³ Kupusa kwa muntu kumawononga umoyo wake ndipo mtima wake umakalipila Yehova. ⁴ Chuma chimapakisa banzako, koma muntu wosauka amachosewa kuli banzake. ⁵ Mboni yaboza sizakangiwa kulangiwa ndipo wokamba vaboza lankhula sazapulumuka. ⁶ Bambili bazapempa chifundo kuli muntu wa bwino ndipo aliwonse ni munzake wa muntu wabwino. ⁷ Babale bonse ba wosauka bamamuzonda; nanga bwanji banzake bamene bayenda patali na eve! Abaitana koma bayenda kudala. ⁸ Wamene apeza nzelu akonda moyo wake; wamene asunga kumvesesa azapeza vabwino. ⁹ Mboni yaboza sizakangiwa kupasiwa chilango, koma wokamba vaboza azawonongeka. ¹⁰ Sichoyenela kuti chofunta kunkala na umoyo wapamwamba makamaka kuti kapolo alamulile mabwana yake. ¹¹ kuziba njila yabwino kuchedwesa kukalipa ndipo ni ulemelelo wake kusaikako nzelu ku milandu. ¹² Mukwiyo wa mfumu uli monga ku uluma kwaka nkalamu ka ng'ono, kuwama mutima kwake kuli monga mame muma uzu. ¹³ Mwana wopusa aononga batate bake ndipo mukazi wokambisisa ali monga manzi yo donya. ¹⁴ Nyumba na chuma ni choloba chochokela kumakolo, Koma mukazi wanzelu achokela kuli Yehova. ¹⁵ Ulesi umangenesa muntu mutulo tukulu, koma wamene safuna kugwila nchito azankala na njala. ¹⁶ Wamene asunga lamulo asunga umoyo wake, koma muntu wamene sasunga njila zake azafa. ¹⁷ Wamene akomela mutima muntu osauka amakongolesa kuli mulungu ndipo azamubwezela vamene achita. ¹⁸ Langa mwana wako pamene chiyembekezo chikalipo ndipo musayambe chabe kufunisisa kumupaya. ¹⁹ Muntu waukali afunika kumupasa chilango; ngati wamupulumusa, ufunika kubwezapo futi kachibili. ²⁰ Mvelela upungu na kumvelela malangizo, kuti pakusiliza pakayena unkale na wanzelu. ²¹ Maganizo niyambili mumutima mwa muntu, koma lingo ya mulungu ndiye yamene iza imilila. ²² Kukulupilika ni vamene muntu amafunisisa ndipo wosauka aliko bwino kuchila waboza. ²³ Ulemu wa Yehova umapeleka bantu ku umoyo; aliwonse wamene ali nacho azakutula ndipo sazafikiliwa na chili chonse choipa. ²⁴ Waulesi amashika kwanja yake mu mbale; sazaibwezapo olo kukamwa kwake. ²⁵ Mumenyeni wonyozela, ndipo muntu wopusa azankala wochenjela; Langa wamene aziba ndipo azankala na kuziba. ²⁶ Wamene abela batate bake na kupisha bamayi bake ni mwana mwamuna wamene amaleta manyazi na manyozo. ²⁷ Mwana wanga ukasiya kumvelela malangizo, uzasoba na kuchoka ku mau yanzelu. ²⁸ Mboni yaboza imanyoza chilungamo ndipo kamwa ya woipa imamela uchimo. ²⁹ Chilango chakonzekelwa bo nyoza kukwapula misana kwa vi puba.

Chapter 20

¹ Vinyo imalengesa chipongwe na moba umalengesa ndewo; Alionse wamene amasobesewa na chakumwa alibe nzelu. ² Kuyopa mfumu kuli monga nkalamu yo buula; wamene amukalipisa aono ga umoyo wake. ³ Kulewa mikangano kumaleta ulemu; Koma chipuba chili chonse chimajumpila kukukangana. ⁴ Waulesi salima ntau ya mvula; afuna pa ntau yokolola, koma sadzapeza kanthu. ⁵ Lingo ya mumutima mwa muntu kuli monga manzi ya patali, koma muntu wamene ali na kumvesesa anaga tapemo. ⁶ Bambili bakamba kuti nibokulupilika, koma nindani angapeze wokulupilika? ⁷ Wolungama amayenda mu ungwilo wake, ndipo bana bake bamene bayenda munjila zake bazadaliska. ⁸ Mfumu yamene inkala pamupando wa ufumu kugwila nchito ya oweluza wamene akamba na menso yake voipa vonse vamene vili kusogolo kwake. ⁹ Ndani anganene, "Nasunga mutima wanga woyela; ndine woyela kuchoka ku uchimo"? ¹⁰ Kulema kosiyanasiyana na mipimo yosiyanasiyana -Yehova azonda vonse. ¹¹ Olo mufana amazibika na vochita vake, ngati nkaliidwe yake niyoyela na kulungama. ¹² Matu yamene yamvela na menso yamene ya yangana Yehova ndiye anapanga vonse. ¹³ Usakondese kugona ndaba ungasauke; segulani menso yanu ndipo muzankala na vakudya vambili. ¹⁴ "nivoipa! nivoipa!" Akamba wogula, koma akachoka ayamba kuzimvela. ¹⁵ Pali golide na myala yambili yodula maningi, koma milomo yanzelu ni mwala wobeka wamtengo wapatali. ¹⁶ Tenga chovala cha muntu wamene achingiliza mlendo, na kuchisunga kunkala chogwililamo akaikila chitetezo mukazi wachiwelewele. ¹⁷ Mukate woipeza munjila yo yipa umveka bwino, ¹⁸ Volingalila vimankazikisiwa na kupasiwa nzelu ndipo na chisogozo chanzelu mukausha nkondo. ¹⁹ Tonzyo imasokolola vobisika, mwa icho osagwilizane na bantu bamene bakamba maningi. ²⁰ Muntu akatembelela batate bake kapena amayi bake, nyale yake izazimiwa pakati pa mudima. ²¹ Cholowa chamene chinapezewa mwamsanga poyamba sichizasila bwino. ²² Usakambe ati, "Nizakubwezela choipa ichi!" Embekeza Yehova didzakubwezerani choipachi." Yembekezerani Yehova ndipo azakupulumusani ²³ Yehova amazondana na mipimo yosiyanana, ndipo sikelo yaboza si yabwino. ²⁴ Mayendedwe ya muntu yamasogolelewa na Yehova; nanga angamvesese bwanji njila zake? ²⁵ Ni msampa ku muntu wokamba mobilimila, "Chintu ichi nichoyela," nakuyamba kukanizila tantauzo ya vamene enze anakamba pambuyo paku lumbila kwake. ²⁶ Mfumu yanzelu imaulusa boipa ndipo izalanga boonse bantu boyipa maningi. ²⁷ Muzimu wa muntu ndiye nyali ya Yehova, yoyaka mukati mwake monse. ²⁸ Chifundo na kukulupilika visunga mfumu; mupando wake wa ufumu unkazikika na chikondi. ²⁹ Ulemelelo wa banyamata ndiye mpamvu zao, na ulemelelo wa nkalamba ni imvwi zao. ³⁰ Makofi yamene yamasiya chilonda yamasuka voyipa na ku menyewa kumapanga vibalo vamukati kutuba.

Chapter 21

¹ Mtima wa mfumu ni mumana wa manzi mumanja mwa Yehova; amaupindamulila kuli konse kwamene kwamukondwelesa. ² Njila ya muntu alionse ni yolungama pamenso pake, koma Yehova ndiye amayesa mitima. ³ Kuchita choyenela ndipo chilungamo maningi nichovomelekezewa kuli Yehova kuchila nsembe. ⁴ Menso, na mutima womeka, nyali ya oipa ni chimo. ⁵ volingalila va muntu wosebenza na mpamvu vimabwelesa vabwino, koma alionse wamene ayendesa kubwela kunkala mpawi. ⁶ Popeza chuma na lulimi yaboza ni chimfwile chamene sichinkalisa ndipo ni msampa wamene upaya. ⁷ Chongo cha boipa chizaba pilikisha, pakuti bakana kuchita chilungamo. ⁸ Njila ya muntu wochimwa niyo benda benda, koma woyela achita chilungamo. ⁹ Kunkala weka pamtenje wanyumba kulipo bwino kuchila ku nkala munyumba pamozi na mkazi wokambisisa. ¹⁰ Njala ya woipa ilakalaka voipa; wamene ankala naye pafupi sama onapo kukoma mtima muli eve. ¹¹ Pamene onyoza alangiwa, wopusa amankala wanzelu, ndipo wanzelu akalangiwa amagwila nzelu. ¹² Wolungama amayanganila nyumba ya woipa, amaleta bantu boipa kuchionongo. ¹³ Wamene avala matu yake kuti asamvele kulila kwa osauka, na eve azalila, koma sazayankiwa. ¹⁴ Mphaso yakabisila ibweza mkwiyo ndipo mpaso yobisika izizilika mkwiyo wampamvu. ¹⁵ Chiweruzo chachilungamo chikachitiwa chimaleta chisangalalo kuli wolungama, koma wamene achita voipa amvesa manta.chitits ¹⁶ Wamene ayenda yenda kuchoka munjila yomvesesa, azapumula mumusonkano wa bakufa. ¹⁷ Alionse wamene akonda kuzisangalasa azankala wosauka; wamene akonda moba mafuta sazankala wolemela. ¹⁸ Muntu woipa nicho ombolelako wolungama ndipo wachiwembu ndiye cho ombolelako bantu bo imilila bwino. ¹⁹ Chilipo bwino kunkala muchipululu kuchila kunkala na mukazi wamkwiyo nakukambisisa. ²⁰ Chuma cha mtengo wapatali na mafuta visungika m'nyumba ya wanzelu; Koma wopusa amamela vonse. ²¹ Wamene achita volungama na wachifundo ndiye apeza moyo na chilungamo na ulemu. ²² Wanzeru amapima munzi wa muntu wampamvu, nakugwesa chipupa chao cholimba chamene benzokulupililamo. ²³ Wamene asunga pakamwa pake lulimi yake azichingiliza ku vovuta. ²⁴ Wozitukumula na wozimvesa zina yake- ndiye wonyoza, Achita mozikuza. ²⁵ Chilakolako cha muntu waulesi chimamupaya, pakuti manja yake yamakana kugwila nchito. ²⁶ siku yonse akumbwila na kulakalaka vambili, koma wolungama apasa mosabweza kumbuyo. ²⁷ Nsembe ya oipa inyansisa; ni chonyansa maningi bakachibwelesa na lingo yoipa. ²⁸ Mboni yaboza izasoba, koma wamene amvela azakamba ntau zonse. ²⁹ Woipa amayumisa pa menso pake, Koma wo ongoka aziba njila zake. ³⁰ Kulibe nzelu, kulibe kumvesesa, ndipo kulibe upungu ungashushane na Yehova. ³¹ Kavalo yakonzekela siku ya nkondo, koma kupambana ni kwa Yehova.

Chapter 22

¹ Mbili yabwino isankiwa kuchila chuma chambili, ndipo chisomo chichila siliva na golide. ² Bantu bolemela na bosauka bali na vinthu vopalana—Yehova ndiye mlengi wa bonse. ³ Wochenjela aona voipa, nakubisama; ⁴ Malipilo yozichepesa ni kuyopa Yehova na chuma, ulemu, na umoyo. ⁵ Minga ni misampa zili munjila ya wosalungama; wamene asunga umoyo wake azankala kutali na beve. ⁶ Punzisa mwana njila yomuyenela, ndipo akakota sazachokamo mu malangizo. ⁷ Wolemela amalamulila osauka ndipo wokongola ni kapolo wa wokongolesa. ⁸ Wamene ashanga kusalungama azakolola voipa na nkoli ya ukali wake izazima. ⁹ Muntu alinalinso ya mutima wabwino azadalisiwa, chifukwa apasako bosauka vakudya vake. ¹⁰ Chosa wonyoza, ndipo ndewo ichoke; kukangana na mwano vizasila. ¹¹ Wamene akonda mtima woyela, ndipo ali namau yachisomo, azankala mnzake wa mfumu. ¹² Menso ya Yehova yayanganisira pali kuziba, Koma amagwesa mau ya woipa. ¹³ Waulesi amakamba, "Muli nkalamu mu njila! n izapaiwa mumalo owonekela. ¹⁴ Pakamwa pa mkazi wachigololo ni chimugodi chitali; Yehova ukali wake wavunduliwa pali aliwonse wamene agwelamo. ¹⁵ Upuba niwomangililiwa mumutima wa mwana, koma mukwapu wa chilango umaupilikishila kutali. ¹⁶ Wamene adyakilila wosauka kuti apakise chuma chake, kapena kupasa bantu bo lemela, azasauka. ¹⁷ Segula kwatu yakoumvele mau ya banzeli ndipo uyike mtima wako pa kuziba kwanga, ¹⁸ pakuti chizawamila iwe ingati uyasunga mkati mwako, ngati yonse yali pa milomo zako. ¹⁹ mwa icho chikulupililo chako chinkale pali Yehova, ine nikupunzisa vamene ivi lelo, olo kuli iwe. ²⁰ Kodi sininakulembele malangizo na vizibiso makumi yatatu, ²¹ kuti nikupunzise chazowona na mau yo yokulupilika aya, kuti mupereke mayanko yokulupilika kuli bamene banakutumani. ²² Usabere wosauka chifukwa chakuti ni wosauka, olo kupwanya bosoba pachipata, ²³ pakuti Yehova azapapatila mlandu wao, ndipo azapoka moyo wa obabela. ²⁴ Usankale na munzako wamene amalamuliliwa na ukali ndipo na wopunda punda chifukwa ch mkwiyo, ²⁵ kuti ungaphunzile njila zake, nakukobewa mumusampa. ²⁶ usankale muntu wovomela kupeleka kapena kulonjeza, kulipilila nkongole muntu, ²⁷ Ngati mulibe ndalama zolipilila, chingalekese muntu winango kukupokabi bedi yanu nichani? ²⁸ Musachose mwala wakudala wamalile wamene makolo yanu yana yika. ²⁹ Uona muntu woziba bwino nchito yake? Azaimilila pamenso pa mafumu; saza imilila pameso pa bantu wamba.

Ecclesiastes

Chapter 1

¹ Aya ndiye mau ya Mupunzisi, mubadwo wa Davide na mfumu mu Yerusalemu. ² "Vachabechabe! Vachabechabe! Akamba Mupunzisi." Vachabechabe! Vonse niva chabechabe!" ³ "Nanga ni mpindu bwanji yamene muntu apeza kuchokela munchito zamene achita pansi pano? ⁴ Mubadwo winangu uyenda , mubadwo winangu ubwela, koma ziko lapansi izankala muyayaya. ⁵ zuba imachoka, nakungena naku tamangila kumalo kwamene imachokela. ⁶ Mpepo imawomba kumwera naku zunguluka kumpoto, kuyenda mozonguluka ntawi zonse munjila yake nakubwelela futi. ⁷ Mimana yonse imatila munyanja, koma nyanja siimazula. Kwamene misinje iyenda , nikwamene yamayenda futi. ⁸ Vonse vimankala volemesa , ndipo palibe wamene angavifotokoze. Linso simakutula navamene imawona, kapena kwatu kukutula navamene imanvela. ⁹ Mwamene chinalili ndiye mwamene chizankalila, na vonse vamene vimachitiwa ndiye vamene vizachitiwa. ¹⁰ Palibe chintu chamanje pansi pano. Nanga pali chinangu chilichonse chamene tingakambe kuti, 'Onani, ichi nichamanje'? Chilichonse chamene chinalipo chinanakhaleko nthawi itali, mumibadwe yamene inabwera kale ife tisanakhaleko. ¹¹ Palibe wamene aoneka monga angakumbukile zamene zinachitika kale, na zamene zinachitika pambuyo pake ndiponso zamene zizachitika pasogolo sizizakumbukiwa. " ¹² Ine ndine Mupunzisi, ndipo nankhala nili mfumu ya Israeli mu Yerusalemu. ¹³ Ninasimikiza mumutima mwanga kuti nibelenge ndi kusanthula mwanzeli zonse zamene zimachitika paziko lapansi. Kusakila kwameneuko ni nchito yolemesa yamene Mulungu apeleka kuli bana ba banthu kuti bankhale otanganikwa nayo. ¹⁴ Naona nchito zonse zochitiwa pansi pano, ndipo onani, vonse vilibe kanthu, ndi mtima. ¹⁵ Zopombeka sizingapombosoke! vosoba sivingabelengedwe! ¹⁶ Nakamba na mutima wanga, nakuti, ona, napeza nzelu zikulu zopambana bonse banali mu Yerusalemu nikalibe kubadwa; mutima wanga waona nzelu zazikulu na kuziba. ¹⁷ Mwaichi ninaika mutima wanga kuti nizibe nzelu komanso misala na kupusa. Ninabwela mukuziba kuti naichi futi chinali choyesa kubeta mphepo. ¹⁸ Pakuti mu nzelu zambili muli zokhumudwisa zambili, ndipo wamene awonjezela chizibiso amachulukisa chisoni.

Chapter 2

¹ Ninati mumutima mwanga, "manje bwela, nizakuyesa na chisangalalo. Sangalalani nazo." Koma onani, ivi vonse vilibe tandauzo. ² Ninakamba pa kuseka, "Nizosokonezeka," ndiponso zosangalasa, "Nganga zingatandize chani?" ³ Ninazifunsa mumutima mwanga mwamene ningakwanilisile zokumbila zanga ndi vinyu. Ninavomeleza maganizo yanga yanisogolele na nzelu ngakhale ninagwililila ku zopusa. Ninali kufuna kuziba zamene zili zabwino kuti bana babanthu bazichita paziko lapansi mumasiku ya umoyo wawo. ⁴ Ninakwanilita vinthu vikulu. Ninazimangia nyumba zanga nakuzilimila minda yamphesa. ⁵ Ninazipangila minda yamaluba na mapaki, na kubyala mitengo ya vipaso vamtundumitundu. ⁶ Ninapanga visime vamanzi votilila nkhalango mwamene mumamela mitengo. ⁷ Ndinagula bakapolo bamuna na bakapolo bakazi; Ninali na bakapolo banabadwila munyumba yanga yaufumu. Ninalinso na ng'ombe zobeta zambili, na zobeta zambili, kupambana mafumu yonse yamene yanalamulila ine nikalibe kunkala mu Yerusalemu. ⁸ Ninazipezela siliva na golide, na chuma cha mafumu na zigawo. Ninatenga oyimba, bamuna na bakazi, na bazikazi bambili, chisangalalo cha bana babanthu. ⁹ Ndipo ninankhala wolemela na wachuma kuchila bonse banakhala mu Yerusalemu nikalibe kubadwa, na nzelu zanga zinasalilila muli ine. ¹⁰ Chilichonse chamene menso yanga yanafuna, sininavisiye. Sininayumise mutima wanga chisangalalo chilichonse, chifukwa mutima wanga unakondwela na nchito zanga zonse na chisangalalo chinali mphotho yanga panchito zanga zonse. ¹¹ Mwaichi ninayang'ana pa zonse nchito zonse zamene manja yanga yanachita, na nchito zamene ninagwila, koma futi, vonse vinalibe pindu-monga chabe kutamangisa mpepo. Panalibe pindu paziko lapansi. ¹² Pamenepo ndinatembenuka kuti nione nzelu, na misala, na usilu. Kodi munthu wina wamene azankala mfumu wosatila angachite chani kupambana zamene mfumu inachita kale? ¹³ Mwaichi ninayamba kuziba kuti nzelu zili na phindu kuchila kupusa, monga mwamene kuunika kuli bwino kuchila mudima. ¹⁴ Munthu wanzelu amagwilisa nchito menso yake pamutu kuti aone kwamwene ayenda, koma wopusa amayenda mumudima, ngankale aziba kuti zamene niziba kuti zochitika kuli bonse. ¹⁵ Ndipo ninakamba mumutima mwanga, "Chamene chimachitika ku opusa, chizachitika kuli ine. Nanga vimasiyana bwanji nikankhala wanzelu kwambili?" Ninamaliza mumutima mwanga, "Nazamene izi zilibe matantauzo." ¹⁶ Pakuti wanzelu munthu, monga wopusa, samakumbukiliwa ku nthawi yayitali. Mumasiku yobwela vonse vizaibalika. Munthu wanzelu amafa monga mwamene amafela wopusa. ¹⁷ Mwaichi ninanyasidwa na umoyo chifukwa nchito zilizonse paziko lapansi zinali zoipa kwa ine. Ichi nichifukwa chakuti vonse vinalibe pindu-monga kutamangisa mphepo. ¹⁸ Ninazonda nchito zanga zonse zamene ninagwila paziko lapansi chifukwa nifunika kuzisiya ku munthu wamene abwela pambuyo panga. ¹⁹ Pakuti nindani wamene aziba ngati azankhala wanzelu kapena wopusa? Koma iye azankhala wolamulila vinthu vonse paziko lapansi kuti nchito zanga na nzelu zanga zamanga. Navamene ivi vilibe pindu. ²⁰ Chifukwa chake mutima wanga unayamba kusila nzelu pa nchito zonse ninachita paziko lapansi. ²¹ Pakuti pafunika kunkhala munthu winangu wamene asebenza nchito na nzelu, na kuziba, na luso, koma azasiya zonse zamene ali nazo kuli munthu wamene sanapangepo chilichonse. Naichi futi chilibe pindu — kulibe chilungamo chachikukulu. ²² Nanga munthu amapindula chani na nchito zake zonse na kunjenjemela kwa mutima wake panchito za ziko lapansi? ²³ Siku ililonse nchito yake imankhala yobaba na youlemesa, ndipo usiku muzimu wake siupeza kupumula. Izi nazo zilibe pindu. ²⁴ Palibe chinangu chabwino ku munthu kuchila kudya na kumwa, na kukuta na vabwino vamunchito yake. Ninawona kuti chazooka chimachokela mukwanja kwa Mulungu. ²⁵ Pakuti nindani angadye kapena nindani angasangalale mumutundu ulibonse kulibe Mulungu? ²⁶ Pakuti kuli munthu wamene amukondwelesa, Mulungu amamupasa nzelu na kuziba, na chimwemwe. Koma, amapasa wochimwa nchito yakuti asonkhanise na kusunga kuti apeleke kwa munthu wamene amakondwelesa Mulungu. Ivi vonse vilibe pindu, vii monga kutamangisa mpepo.

Chapter 3

¹ Yangana, Yehova alipafupi nakuchosa vonse muziko yapansi, kuyi ononga, naku yisiya ilibe chintu, na kumwazya bo nkalamo. ² Ivivizabwela, pamuntu aliyense, napaba nsembe, pali akapolo, napama bwana bao; kuli osebenza munyumba, na kuli bwana wake mukazi; kuli wogulisa, na kuli wogula; kuli wokongolesa, nakuli wokongola; kuli wolandila kaloba, na kuli wopasa kalosa. ³ Ziko izawonongewa yonse naku vuliwa; pakuti yehova akamba aya mau. ⁴ Ziko yiyuma naku fota, pansi pa ziko payenda pazimilila, bantu ba pamwanba mwamba ba muiko ba onongeka. ⁵ Ziko ya yipisiwa na bantu bonkalamo chifukwa chakuti siba konka lamulo, baononga ma lamulo, na kuowanya chipangano chamuyayaya. ⁶ Chifukwa cha icho tembelelo ang'amba ng'amba ziko, na bantu bonkalamo bapezeka na mulandu. Bonkala muziko lapansi bapya, na ba ng'ono bantu ndiye basala. ⁷ Vinyu yanyowani iyuma, mpesa zifota, mitima yonse yosangalala ibuula. ⁸ kuvweka kwbwino kwa matambolini kwa leka, na ntungulu za abo bosangala; na chisangalalo cha ma zeze cha zima. ⁹ Basiya kumwa vinyu na kuyimba, na kuli abo bakumwa moba ulula. ¹⁰ Muzinda wa musikonezo wagwesewa; manyumba yonse ya valiwa mulibe na chili chonse. ¹¹ Muli kulila mu njila chifukwa cha vinyu; chimwemwe chonse chinafipisiwa, kuvwela bwino kwa mumalo kwa soba. ¹² Mu muzinda munankala malo yosiwa, na vipata vina pwanyiswa na kuwonongeka. ¹³ Pakuti ndiye mwamene vizankalila pa maziko yonse ya pansi, monga mwamene mutengo wa olivi umenyewa, olo monga mwamene vilili vosalila pokolola mpesa. ¹⁴ Bazakwezeka mau yao pamwamba na kupunda ukulu wa Yehova, na cgisangalalo bazapunda kuchoka mu nyanja. ¹⁵ Chifukwa cha icho ku mawa pasani ulemelelo Yehova, na mumbali mbali ya nyanja pasani ilemeloku zina ya Yehova, mulungu wa israeli. ¹⁶ Kuchokela kuma ziko yakutali ya pa ziko lapansi tamvela nyimbo, "ulemelelo kuli olungama!" Koma ninakamba naonongeka, naonongeka, soka kuli ine! Bonama bachita vintu mukunama; nimwamene, bo nama bachita vo nama mo pitisila." ¹⁷ kuyofya chimugodi, na vo teya vili pali imwe, bonkal pa ziko lapansi. ¹⁸ Wamene ataba chongo choyofya azagwela mukati mwamugodi, na uyo wamene achoka pakati oachimugodi azagwiliwa na vo teya. Mawindo ya kumwamba yaza seguliwa, na maziko yapa ziko lapansi yaza nyang'anya. ¹⁹ Ziko yapansi izapwanyikilatu, ziko izang'ambika ng'ambika; ziko izanyang'anyisiwa na mpavwu. ²⁰ Ziko yapansi izazezeleka monga muntu wokolewa ndipo izabwelela kumbuyo na kusogolo monga kanyumba kamauzu. Uchimo wake uzamulemela na kugwa na kusanyamuka futi. ²¹ Pasiku ija Yehova aza langa bankala munyumba ili kumwamba, nama mfumu yama ziko ya paziko yapansi. ²² Bazasonkanisiwa pamozi, bomangiwa mu mumuondi, nakuvaliliwa mujele; ndipo pakapita masiku yambili bazapasiwa chilango. ²³ Elo mwezi uza mvela nsoni, na zuba iza sebanyika, pakuti Yehova wa makamu aza lamulila pa pili la ziyoni namu yelusalemu, na pamenso pa bakulu bake mu ulemelelo.

Chapter 25

¹ Yehova, ndiwe mulungu wanga; nizakukweza, nizatamanda zina yak; chifukwa wachita vintu vabwino, vintu unakonzeka kudala, mu chikulupililo chofikapo. ² Pakuti mwapanga muzinda kuunjikika, wa vipupa volimba, kuonongeka, na wo chingiliza balendo mukusiya kunkala muzinda. ³ Mwaicho bantu bampavwu bazakulemekeza; muzinda wa maziko yankanza yazakuyopa. ⁴ Chifukwa wankala malo ya chitetezo cha ovutika, monkalamo kuli osoba mukuvutika kwake, monkalamo kuli chimpepo chikulu na chinfwilie kuli mulilo. Pamene mpeya ya bankanza inali monga chimpepo chikulu ktsusana chiumba, ⁵ ndipo monga kupya mu malo yoyuma, muna gonjesa chono cha balendo, monga kupya kugonjeseka na chifwile cha kumbi, nimwamene nyimbo ya bankaza iyankiwa. ⁶ Palupili iyi Yehova wa makamuazapangila bantu bonse pwando ya vintu voina, ya vinyu yosanka, yoa nyama yofeba pali banyamata. ⁷ Azaononga palupili iyi vichingilizila pali bantu bonse, chitetezo chovilinkila maziko yonse. ⁸ Azamela infa muyayaya, ndipo ambuye Yehova zapukuta misozi za bantu bonse kuchokela pa menso pawo; kusenyka kwa bantu bake azachosapo pa ziko yapansi yonse, pakuti Yehova achikamba. ⁹ Kuzka kambika pa siku ya, "Ona, uyu ni mulungu watu; tamuyembekezela eve, ndipo azatipulumusa. Uyu ni Yehova; tamuyembekezela eve, tizakondwelela na kusangalala mu chipulumuso chake." ¹⁰ Chifukwa pa lupili iyi kwanja ya Yehova izapumula; ndipo Moabu azadyakiwa pansi mu malo yake, monga mwamene mpasa idyakiwa pansi mu mugodi ozula na manyuwa. ¹¹ Bazatambusula manja yawo pakati pake, monga onyaya amatambusula manja yake kuti anyaye. Koma yehova azbweza pansi kuzinvesa kwawo ngakale ukaswili wa manja yawo. ¹² Vipupa vanu vitali vozichingilizamo azazigwesa mpaka pansi, ku kalukungu.

Chapter 26

¹ Tsiku lomwelo adzaimba nyimbo iyi m'dziko la Yuda: Tiri ndi mudzi wolimba; Mulungu wapanga chipulumutso malinga ake ndi linga lake. ² Tsegulani pazipata, kuti mtundu wolungama womwe umasunga chikhulupiriro ukalowe. ³ Malingaliro omwe amakhala pa inu, mumusunga mumtendere wangwiro, chifukwa amakukhulupirirani. ⁴ Khulupirirani Yehova kwamuyaya; pakuti mwa Yehova ndiye thanthwe losatha. ⁵ Pakuti adzagwetsa iwo akukhala modzikiza; mzinda wokhala ndi mpanda wolimba kwambiri adzaugwetsa, uugwetsera pansi. adzaligwetsa fumbi. ⁶ Adzapondaponda ndi mapazi a anthu osauka ndi kupondereza aumphawi. ⁷ Mayendedwe a olungama ndi olungama, Olungama; uongola mayendedwe a olungama; ⁸ Inde, panjira ya ziweruzo zanu, Yehova, ife tikuyembekezerani; dzina lanu ndi mbiri yanu ndizofunitsitsa zathu. ⁹ Ndakulakalaka usiku; inde mzimu wanga wakufunafuna. Pakuti maweruzo anu akafika padziko lapansi, okhala m'dziko lapansi adzaphunzira chilungamo. ¹⁰ Woipa acitidwe cifundo, koma sadzaphunzira cilungamo. M'dziko lowongoka amachita zoipa ndipo saona ukulu wa Yehova. ¹¹ Inu Yehova, dzanja lanu lakwezedwa, koma iwo sakudziwa. Koma adzaona changu chako kwa anthu ndi kuchita manyazi, chifukwa moto wa adani ako udzawatha. ¹² Inu Yehova, mudzatibweretsera mtendere; pakuti mwakwaniritsanso ife ntchito zathu zonse. ¹³ Yehova Mulungu wathu, ambuye enanso osatinso adatilamulira; koma tikutamanda dzina lanu lokha. Iwo anafa, sadzakhalanso ndi moyo. ¹⁴ adafa, sadzauka. Udabwera kudzaweruzo, ndipo udawawononga, ndi kuwononga chikumbukiro chawo. ¹⁵ Mwachulukitsa mtundu, Yehova, mwachulukitsa mtundu; ndinu olemkezeke; mudakulitsa malire onse adziko lapansi. ¹⁶ Yehova, iwo akuyang'anira Inu nsautso; adanong'oneza mapemphero pamene chilango chanu chinali pa iwo. ¹⁷ Monga mayi wapakati amayandikira nthawi yoti abereke, atakhala ndi zowawa ndikufuula ndi zowawa za pobereka, momwemonso takhala pamaso panu, Ambuye. ¹⁸ Takhala ndi pakati, takhala tikumva zowawa, koma zimakhala ngati tangobala mphepo. Sitinabweretse chipulumutso padziko lapansi, ndipo anthu okhala padziko lapansi sanagwe. ¹⁹ Akufa anu adzakhala ndi moyo; mitembo yawo idzauka. Dzukani ndipo imbani mwachimwemwe, inu okhala m'fumbi; chifukwa mame ako ndi mame a kuwala, ndipo dziko lapansi lidzatulutsa chakufa chake. ²⁰ Lowani anthu anga, lowani m'zipinda mwanu, nimutseke pamakomo panu; bisalani kanthawi pang'ono, kufikira mkwiyo utadutsa. ²¹ Pakuti taonani, Yehova ali pafupi kutuluka m'malo mwake kulanga okhala padziko lapansi chifukwa cha mphulupulu zawo; dziko lapansi lidzavundukula mwazi wake, ndipo silidzabisanso ophedwa ake.

Chapter 27

¹ Pasiku ija yehova nalupanga yake yolimba, ikulu nayo yofya azalanga leviatani njoka yoyenda monyonga, leviatani yamene ili munyanja. ² Musiku ija; munda wampesa wa vinyu, uimba paichi. ³ "Tne, Yehova ndine ochingiliza; nimai tilila ntawi zonse. Nima londa usiku na mu zuba kuti aliyense asai ononge. ⁴ Sindine okalipa, O, kuti panali mitungwi na minga! Munkondo nizabakonka; nizabashoka bonse pamozi; ⁵ Koma ngati batenga chitetezo changa naku panga mutendele naine; lekani bapange mutendele naine. ⁶ Pa siku yamene ibwela, Yakobo azatenga mizyu; israeli azapukilanaku choka; baza zuzya pansu navi paso." ⁷ Nanga yehova amenyana na Yakobo na israeli monga mwamene ana menyana na maziko yamene yanamenyana nabo? Nanga bapaiwa Yakobo na israeli monga mwaku jubiwa kwa ayo maziko yamene yana paiwa nabeve? ⁸ Muchimo chimozi chamene mwapikisana, kupisha Yakobo na israeli; anabapisha nakupema koipa pa siku yampepo yaku mazulo. (mumalo mwama yeso wolinga yambili masulidwe yamanje yaliko na ganizo yamene ipalanako kubapishasha) ⁹ Munjila iyi, machimo ya Yakobo yafafaniziwa, popeza ichi chizankala chipaso chonse chochosa chimo yake: pamene azapanga myala za guwa ngati choko naku imowanya muma gawo, ndipo kuzankala kulibe choimilila pali ma mitengo ya Ashela kapea nonunkilisa pa guwa. ¹⁰ Popeza muzinda wochingiliziwa ulipa weka, monkalamo mwasiwa nakutaiwa monga chipululu. Kuja ka ng'ombe kang'ono kazidyesa naku gona nakudya ntambi zake. ¹¹ Pamene ntambi zayumo, ziza pwanyika. Bazimai baza bwela nakuzipangila nkuni, popeza sibantu bonvesesa. Mwaicho mulengi wabo saza ba chitila chisoni, nawamene ana bapanga sazabanvelela chifundo. ¹² Chizabwela kuti pasiku ija kuti yehova azamwaza kuchokela ku musinje wa yufuletisi kufikila ku wadi mu egupito naimwe, bantu ba israeli, muza fakiwa pamozi umozi umozi. ¹³ Pasiku ija lipenga ikulu izakaliziwa; nabo vutisiwa mumalo ya assiria bazakabwela, nabo pishiwa malo ya egupito. Baza kampeza Yehova pa pili yoyela mu yelusalemu.

Chapter 28

¹ Soka kuli korona yo zivesa yamene ivaliwa na aliyense chakolwa waku Efraimu, na maluba yosilila yake ya ulemelero ya bwino, korona yamene yaikidwa pa mutu pa chikwa cha abo bamene ba pambana vinyu! ² Onani, Ambuye atuma umozi wamene nimukulu na olimba; monga chipeco chama talala na chipeco cho ononga, monga mvula yamene iyenda na manzi yotaiikila; ndipo azataya korona iliyense pansi. ³ Ma korona yo zivesa yama chakolwa yaku Efraimu yaza dyakiwa pansi pa kwendo. ⁴ Kusilila kwa maluba yake ya ulemelero wa bwino, yamene ali pa chikwa yolemela, izankala monga mukuyu woyamba wakupya kukalibe kupya, kuti, ngati aliyense aka uwona, pamene ukalibe kunkala mumanja mwake, aza utunyila pansi. ⁵ Musiku ija Yehova wamakamu azankala korona wabwino na cha ufumu chapa mutu cha bwino chaku kumbusa bantu bake, ⁶ muzimu wachi lungamo wa uyo amene ankala pa chiweluzo, na phavu kuli abo bamene ba bweza ba dani bao pongenela pabo. ⁷ Koma na bamene abo bakumwa chokolewesa cha vinyu, na kuzezeleka na vokumwa va phavu. Wa sembe na muneneli wamene akamwa chokolewesa na vokumwa va phavu, ndipo baza melewa na vinyu. Bazezeleka na vo kumwa va phavu, kuzezeleka mu maso penya naku kagiwa kupanga maganizo bwino. ⁸ Zoona, ma ntebulo yonse yaza mbisiwa nama lusi, kuti kulibe na malo ya bwino. ⁹ Nikuli ba ndani kwamene aza phuzisa nzelu, na kuli ba ndani kwamene aza fotokozela utenga? Kuli abo bamene ba yamwa kapena kuli abo bamene bachosewa ku maziba? ¹⁰ Pakuti chili pa lamulo pa lamulo, lamulo pa lamulo; kulamulila pa ku lamulila, ku lamulila pa ku lamulila; pano kangono, paj kangono. ¹¹ Mwaicho, namilomo yonyoza na lilime ya chilendo aza kamba kuli bantu aba. ¹² Kudala anakamba nabo "uku ndiye kupumula, mupaseni uyo wolema kupumula; ndipo uku ndiye kusisimusiwa, koma sibana nvele. ¹³ Ndipo mau ya Yehova yazankala kwa beve lamulo pa lamulo, lamulo pa lamulo; kulamulila pa ku lamulila, kulamulila pa ku lamulila; pano tugono, paja tugono ndiye kuti bakayenda na kugwela chaku mbuyo, naku pwanyika, kuteya naku gwiliwa. ¹⁴ Ndipo nvela ku mau ya Yehova, iwe wamene unyoza, iwe wamene ulamulila bantu bali mu Yelusalema. ¹⁵ Ichi chiza chitika chifukwa una kamba, "Tinapanga chipangano na imfa, na manda ndipo tafika paku vomelezana. Pamene chikondwelelo chamu kwapu chipita, sichiza tifikila ise. Pakuti tapanga boza mo pumulila, naku tenga monkala muchinyego." ¹⁶ Chifukwa Ambuye Yehova akamba, "Onani, nizaika mu Ziyoni mwala pa maziko, mwala omangiwa, mwala wo oneka bwino, maziko wokazikika. uyo wamene akulupililamo saza nvela manyazi. ¹⁷ Niza panga chilungamo mutengo opimilako, na chilugamo chopimilako. Kupunda kuzapyanga kombisamila kwa boza, manzi yosefukila yazazulila malo ombisamilamo. ¹⁸ Chipangano chako na imfa chizasila naku vomeleza kwa manda sikuza imilila. Kapena pamene manzi ya phavu yapitamo, chiza kundabwisa iwe. ¹⁹ Pamene ipitamo, izakudabwisa iwe, ndipo kuseni na kuseni izapitamo, siku na usiku iza bwela pamene utenga uzaveka, izachitisa manta. ²⁰ Pakuti pogona nipagono kuli muntu kuti aziyondolele, na voyambata nivi gono kuti azi vinikile iye mwene." ²¹ Yehova azanyamuka pa phili ya Perazimu; aza zinyamula kuchita chito yake, chito yake ya chilendo, naku gwila chito ya chilendo. ²² Manje chifukwa ichi musa nyoze, kapena kugwilizana kwanu kuza matila. nina nvela kuchoka kwa Ambuye Yehova wamakamu, pa kukamba kwa chionengeko chapa ziko lapansi. ²³ Ikako nzelu naku vesesesa liu yanga; unkale wo vesesesa ku mau yanga. ²⁴ Kodi mulimi amene alima siku lonse kuti akashange, amalima chabe pansi? Kodi ama pitiliza kupwanya pamwamba naku koza mu munda? ²⁵ Pamene akonza munda, kodi samwaza mbeu yamaluba yowamisa, kushanga cumini, aika tiligo mu mizela na barle mu malo ake oyenela na kutila mumbali? ²⁶ Mulungu wake amamulamula; amamupunzisa mwanzelu. ²⁷ Komanso, mbewu za cara sizipunthidwa ndi ulusi wa zida zamtengo wapatali, kapena kugugudubuza gudumu pamwamba pa chitowe; koma caraway amenyedwa ndi ndodo, ndi chitowe ndi ndodo. ²⁸ Tirigu amapunthira buledi koma osati wotsika kwambiri, ndipo ngakhale mawilo a galeta lake ndi mahatchi ake amabalalitsa, akavalo ake samaphwanyanya. ²⁹ Izinsu zimachokera kwa Yehova wa makamu, amene ali wopambana m'malangizo ake, ndi wanzeru zopambana

Chapter 29

¹ Soka kuli Ariel, Ariel, malo yamene Davide anankala pilizabi chaka ndi chaka; lekani mapwando yazi nkalako mokonkana. ² Koma niza zinguluka Arieli, ndipo ba zayamba kulila na kumvesa chisoni. Ndipo ba zankala kuli ine monga Arieli. ³ Niza kuzinguluka iwe mbali yonse ndipo niza ku bisamila iwe kuku pangila mupanda, ndipo nizaika nchito zoku ganizila za nkondo kususa iwe. ⁴ Uza gwesewa pansi ndipo uzakamba pamene wagwesewa pansi; mau yako yazankala ya pansi kuchokela ku doti. Liwu yako iza mveka ngati muzimu wamene ukamba kuchokela pansi pa doti, ndipo kunja kwa foti yako iza kamba pangono. ⁵ Bantu ba mbili bamene ba mafuna iwe baku kukugwesa, ba zankala ngati muchanga wosefewaa, ndipo ba mbili ba ntota ba zankala semu vopepetewa vimene vi uluka nakupita. Vizachitika maje manje, pangono chabe. ⁶ Yehova wamakamu azabwela kuliimwe na chongo cha mvua, chivomezi, chongo chikulu chimpepo cholimba na mvula yakaleza, ndipo nakuyaka kwa mulilo washoka. ⁷ Zidzakhala ngati loto, masomphenya a usiku: Gulu lalikulu la mitundu yonse lidzamenyana ndi Arieli ndi malo ake achitetezo. Iwo adzamuukira ndi malinga ake kuti amuthamange. ⁸ Zidzakhala ngati munthu wanjala alota kuti akudya, koma akadzuka, m'mimba mwake mulibe kanthu. Zidzakhala ngati munthu waludzu atalota kuti akumwa, koma iye podzuka, akukomoka, ndi ludzu lake losatha. Inde, chomwechonso chiwerengero cha mayiko omwe adzamenyane ndi Phiri la Ziyoni. ⁹ Dabwani mweka ndipo dabwani; kalani mpofu mweka nakunkala ba mpofu! nkalani bokolewa, noti na vinyo; zezeleka, noti na moba. ¹⁰ Pakuti Yehova atila muzimu wake pali iwe muimu wogona tulo maningi. Anavala menso, aneneti, na winikila mitu zanu, nabo ona. ¹¹ Chivumbuluso chonse chankala kwa iwe mau amu buku yamene siyana seguliwe naku pasiwa. ¹² Ngati buku ya pasiwa muntu chamenr saziba kubelenga, "Belenga ichi, akamba kuti, "Siniza belenga." ¹³ Ambuye bana kamba kuti, Äba bantu ba bwela pafupi naine na makamwa na ulemu pa milomo zabo, koma mitima yabo ili kutali na ine, ulemu wamene ba nipasa ni malamulo ya bantu yamene ba napunzila. ¹⁴ Mwaicho, yangana, niza piliza kuchita chintu chodabiwsa pakati pa aba bantu, chodabisa pachu dabwisa, nzelu za bantu babo banzelu baza sila, naku nkala nacho chizibiso. ¹⁵ Soka kuli benve bamene ba biisa ma pulani yochokela kuli Yehova; ndipo na vamenye bachita vili mumudima. ba kamba, "Nindani amene atiyangana, niba ndani bamene batiziba? ¹⁶ Upindamula vintu kuchokela pa mwamba na pansi kansi bowumba doti banga lingane na doti, kuti chitnu chamene ba umba chinga kambe kuti "Sibanani bumbe ine"pa vintu vonse panga iye, İye sama mvesesa"? ¹⁷ Paika ntai kangono, Lebanoni aza sanduliwa munda, ndipo munda uzankala sanga. ¹⁸ Pasiku lija bamene siba mvela mumatu yabo bazanvela mau yamu buku, ndipo menso yaba mpofu yaza ona kuchokela mumudima wawu kulu. ¹⁹ Nabo botitikishiwa bazakondwela futi muli Yehova ndipo bosauka pakti pabo baza kondwela kuli oyela wa Isilayeli. ²⁰ Boyipa bonse baza leka, nabo paya ba zasoba nabonse bamene bachita zoipa, baza chosewapo. Iye na mua apanga muntu kunkala wosusa. ²¹ Bamu pamuteya abo bamene bafuna chilangamo pa mulyango ndipo bogwesa pansi bolungama na boza yabo ilibe kantu. ²² Izi ndiye zamene akamba Yehova ku nyumba ya Yakobo-Yehova, amene anapuluma Abrahamu, "Yakobo sazanvela nsoni, olo pamenso pake sipazagwa. ²³ Pamene aona bana bake, nchtio ya manja yake, baza lengesa zina langa kunkala loyela. Baza lengesa kuyela zina la oyela wa Yakobo naku yimilila boyaka ba Mulungu waba Isilayeli. ²⁴ Abo bamene ba lakwa mumuzimu baza peza kumvesesa, bodandaulo baza punzila nzelu.

Chapter 30

¹ "Soka kwa bana bamene baukila," Yehova anenela. "Bapanga maganizilo, koma siyachoka kwaine; apanga mugwilizano namaziko yenangu, koma sibauziwa nazimu wanga. bafakapo chimo pa chimo. ² Bamayenda ku Igipito pansi koma, sibapempe njila yanga. ayesa kumpempela kuchingilizwa kuli Falao ndi kuchingilizwa mu chinuliki cha Igipito. ³ Kuchingilizwa na Falao ndiye manyazi yanu, ndi chingilizwa kwa mu Igipito muchim nfwile, ndiye kusebnika kwanu, ⁴ olo bana ba mfumu ali pa Zowani ndi otumikila babo banabwela ku Hanesi. ⁵ Bonse bazamvela manyazi chifukwa cha bantu bamene sibanga ba tandiza, bamene sibatandiza bazanvela koma nsoni, na manyozo. ⁶ Kusimikiza za nyama yaku Nagevu: kupitila mumalo muli babvuto na voyofya, nkalamu ikzai na imuna, chipili na njoka zofyoka zombululuka, bananyamuka chuma chabo pa misana ya mabulu na ndalama pa ntunda ya kameli, kuli bantu bamene sibanga bandize. ⁷ Chifukwa ntandizo ya Igipito ilibe nchito mwaichi namutana Rahabu, nkala chbe. ⁸ Manje yenda, lembela pamaso pachi mwala cholembapo, chilembe chimwala, isungike masiku yakusogolo izantala ngati mboni. ⁹ Aba ndiye bantu bamene bopanduka, bana ba boza, bana bamene simanvera malangizo ya Yehova. ¹⁰ Bakamba kuba neneri, "Osaona," ndi ma profita, "osanera zazo-ona kwa ise; koma kukamba mau otiyamikila ise. ¹¹ Choka kumbali yanjila, choka munjila chifukwa mwalengesa woyela wa Isilayelu akamba mosiliza panu yanu. ¹² Ndipo Mulungu woyela wa Isilayela akamba, chifukwa mwakana mau awa nachichetekela ukali wopitikila naku namiwa mwangolapo, ¹³ Iyi chimo izankala kuli iwe, chintu chopwanyika chamene chifuna kugwa monga chintu chonkala chipupa chitali chizagwa mwazizi mwamusanga. ¹⁴ Azachipannya monga mwamene apwanya wopanga mpoto; Sizachisiya pasapezeke tosala tojubika-jubika twamauzu tazapoyewa kulilo olo kutaiwa ba choikamo manze. ¹⁵ Ichi ndiye ambuye akamba woyela wa Isilayeli, mukubwela nakupumula muzapulu musiuu, muzankala zi, muchetele muzalimbisiwa koma simwenze wofuna. ¹⁶ Mukamba kuti, Iyayi, 'pakuti muzambululukila mumahose yanu ndipo muzambululukila mpaka muzakwela yona.... mwamusanga muzaya.... mwamusanga. ¹⁷ Bali 1000 baza taba kuyopa; kwa manta pakufya kwa bantu bali ma..... muzantawa paka wosalo bazayimulila monga myala yoimili pa mwamba pa..... ¹⁸ Ndi Yehova azayembekeza kwa iwe, ndipo odala ayembezele kulangiza chifundo. Pakuti Yehova ndiye Mulungu wachilungamo nichodala na bonse wondila kwa iwe. ¹⁹ Pakuti muntu anaka mu Zayoni, Yelusalemu sazalila nafuti. Azankala nachifundo kwa iwe pakulila kwako. Pamene azanvela aku yanka iwe. ²⁰ olo yehova akupani mukate wamuntawi yovutisa ndi manzi yamu manzi yamutawi yamasauso mwamene bopmuzisa wanu sazabisama nafuti, koma muzaba ona bompuzisa nameso yanu. ²¹ Makutu yanu yazamvela mau kumbuyo kwanu, yamene yakamba kuti iyi ndiye njila, yoyendamo ngati wapindanuka kuzanja lamanja olo kuzanja lamazela ²² Pamene apo muzatenga tumilungu twina twaboza yoftidwa pamozi na Siliva, na golide ndipo muza wataina ngati zinyalala uzabauza bene chokankoni uko. ²³ Azapasa mu ula kwa mbeu zanu yamene uzashanga pansi, ndi mukate wambili wochokela danka ndi mbeu izankala yambili, musiku uja. Ng'ombe zizadya modyelamo nkuku. ²⁴ Ng'ombe ndi bulu, zamene zilima, zizadya zantawi, zameneyo yamene ntengewa na shavelo na foloko. ²⁵ Palupili ili yinse yapa mwamba, paza nkala tumimana twa manzi masiku lila. kunkala kujuba kwakulu zomangilwa utali vizagwa. ²⁶ Kuyaka kwa mwezi kuzankala monga kuyaka kwa zuba ndi kuyaka zuba yimayankika masiku 7 monga Yehova azamanga kuwanika kwa bantu bake nakupolesa kukweshuleka kwa zilonda zabo. ²⁷ Ona, zina la Yehova ichokeka patali apo patali, kufya kwa ukali wake ndi kulema kwa chsi. Milimo yake yiyozula mukali ndi lulimi yake minfga mulilo owononga. ²⁸ Kupema kwake kuli monga chimpepo chachila chamumana chontha monga mumana pakati pa mukosi kusiyanisa maziko na yondolola bowonongeka. Kupema kuli monga kumwamba mkamwa ba bulu kuli bantu nakupanha to chokapo. ²⁹ Uzankala na nyimbo usiku. Pa,eme madyelelo oyera izachitika, nakodwa muntima pamene winangu ayenda natomitililo kupiri ya Mulungu Yehova ku mwala wa Isilayeli. ³⁰ Yehova azapanga kuwala kwakulu na mau yake yazamveka. naukali wake na mulilo woyanka nachimpepo chachikulu na mvula ikulu ya matala. ³¹ Pa mau ya Yehova, Asiliya azaonongela ndi bamenya na ndodo yake. ³² Kukwapula kulikonse kusankanizika kwa iyo. zizankala pamozi natoliza twatolilo pamene bamenyana nabo. ³³ Malo oshokelamo anakonzewa kudala pantawi ya kumbuyo inde anapangilwa mfumu, ndi Mulungu apanga kuli chikulu choy pansi moto unaunjikwa kale na nkuni zambili, kupema kwa Yehova, kuli monga mulilo ukulu uzayaka monga mulilo.

Chapter 31

¹ Tsoka kwa iwo amene apita ku Aigupto kukathandizidwa ndi kudalira akavalo, ndi kukhulupirira magaleta (pakuti achulukadi) ndi apakavalo; Koma alibe nkhawa ndi Woyera wa Israeli, komanso safuna Yehova! ² Komabe iye ndi wanzeru, ndipo adzabweretsa tsoka ndipo sadzabweza mawu ake. Adzaukira nyumba yoyipa, ndi otsutsana nawo amene achimwa. ³ Aigupto ndi munthu osati Mulungu, akavalo awo ndi nyama osati mzimu. Yehova akadzatambasula dzanja lake, mthandizi adzapunthwa, ndipo womathandizidwayo adzagwa; onsewo adzawonongeka pamodzi. ⁴ Atero Yehova kwa ine, "Monga mkango, ngakhale mkango wamphamvu, ukubangula pa nyama yake yodulidwa, pamene gulu la abusa liziitana, koma silimanjenjemera ndi mawu awo, kapena silithawa mawu awo motero Yehova wa makamu adzatsikira kukachita nkhondo pa phiri la Ziyoni, pa phiri lija. ⁵ Monga mbalame zouluka, momwemo Yehova wa makamu adzatchinjiriza Yerusalemu; adzateteza ndi kupulumutsa pamene adutsa ndi kuisunga. ⁶ Bwererani kwa iye amene mwapatuka kwambiri, inu ana a Israeli. ⁷ Pakuti tsiku lomwelo adzachotsa yense mafano ake a siliva, ndi mafano ake a golidi, amene manja anu anachimwa. ⁸ Asuri adzaphedwa ndi lupanga; lupanga losagwira munthu lidzamutentha. Iye adzathawa lupanga, ndipo anyamata ake adzawakakamiza kugwira ntchito yolemetsa. ⁹ Iwo adzataya chidaliro chonse chifukwa cha mantha, ndipo akalonga ake adzaopa pamaso pa mbendera ya Yehova, ati Yehova, amene moto wake uli m'Ziyoni, ndi woyatsa moto ali m'Yerusalemu.

Chapter 32

¹ Onani, mfumu iza lamulila muchilungamo na bana banfumu azalamulila mu chilungamo. ² Bali bonse bazankala mobisamakumpepo naku chimpepo, monga tumimana mumalo oyuma, monga mtunzi wa chimwala chikulu muziko lolema. ³ Ndipo menso yabo bonse bamene ba ona siyazaleka kuona, na matu yabo bonse bomvela bazanvesesa. ⁴ Botamangela bazaganiza bwino namoziba ndipo bachibwibwi bazakamba bwino mosavutika. ⁵ Bopusa sibazabaitana kunkala olemkezeke, nabo bonama sibaza itaniwa olemkezeke. ⁶ Bopusa bakamba kuipa. Baganiza zoipa mumutima zabo, na machitidwe yamene mulibe Mulungu, na kukamba voipa pali Yheova. Amene alengessa ba njala kunkala balibe chilichonse, naba mene bali nachila chamanzi kunkala balibe chamene bazamwa. ⁷ Njila za bantu bonama nizoipaa, babwelesa nzelu zoipa kugwesa bosauka na boza yabo, olo osauko akambe va zo-ona. ⁸ Koma muntu olmekezeke amapanga mapulani. ⁹ yolemekeza; kamba kamachitidwe yolemekezeke aza imilila. Nyemukani, imwe bakazi bankala chabe bana bakazi bamene simusamala nvelani kwaine. ¹⁰ Paka ntawi kangono no pitilapo pa chaka chikulupililo chako chiza onongeka, imwe bakazi bamene simusamala, pakuti kukolola kwa mpesa kuzalepeleka, naku sankana pamozi sikuza bwela. ¹¹ Tutumani, imwe bakazi bamene simuchita chili chonse kalani ovutisiwa bo kulupilila bam; vulani zovala zanu zabwino ndipo osasala nachili chinse valani masaka naku naku zingulusa mumusana. ¹² Uzalila mosalekeza pa minda zabwino, pa mpesa za zamene zibeleka zipaso zabwino. ¹³ Ziko ya bantu banga izamela maningi mitengo za minga nama briers, na monse muma nyumba munali kukonddwela mumuzinda wachikondwelelo. ¹⁴ Nyumba yonkalamo mfumu izaka kaniwa, mizinda wotitkana uzankala ulibe bantu; na lupili na tawa viza nkala mpako mukati ka myala yokulupili muyayaya, chimwemwe chama bul yamusanga, musipu wa gulu; ¹⁵ kufikila muzimu utaikile pali ise kuchokela ku mwamba, ndipo chipululu chizankala munda wabala vipaso ndipo munda wobala zipaso uli monga sang. ¹⁶ Ndipo chilungamo chizankala muchipululu; na chilungamo chizankala mumunda wobala zipaso bwino. ¹⁷ Nchito ya chilungomo izankala mutendele; zotuluka zachilungamo. kusa kamba na chikulupililo muyaya. ¹⁸ Bantu banga bazankala mumutendele; mumanyumba yochingilizwa, na mumalo mopimulila mulibe chongo. ¹⁹ Ngankale mvula ya myala ya wononga sanga yamitengo, na muzinda kuonongekelatu, ²⁰ uza dalisiwa ngati wa shanga mbewu yako mumbali yakamumana kalikonse ndipo lekai kwendo kwa ngombe na bulu kunkala patali.

Chapter 33

¹ Soka kwaimwe, wo-ononga bamene mukalibe kuonongwewa! Soka kubogulisa banzawo benve sibanabapeleke! Ngati mwasiya kuononga, muza onongewa ngati mwaleka kugulisa banzanu, bazaka kugulisani imwe. ² Yehova, nkalani bachifubda kuli ise, tiku yembekezani imwe; nkalani kwanu yatu kuseni kuli konse, chipulumuso chatu pa ntau ya mavuto. ³ Pa chongo chikulu bantu bataba; ngati mwanyamuka, maziko yama mwazikana. ⁴ Vo-onogeka vanu vaikiwa pamozi munga mwamene ntente zimankalila pamozi munga mwamene ntente zimadyela, bantu baza zida. ⁵ Yehova niwapamwamba. Ankala mumalo yapa mwamba. Aza zulisa Zayoni nachilungamo nakuyela. ⁶ Azankala po dalila muntawi yako, chipulumuso chambili, chizindikilo, na nzelu; kuyopa Yehova ndiye chuma chake. ⁷ Onani, botumiwa babo balila munjila; bolemekezeka bamene bayembekezela mutendele balila manigni. ⁸ Munjila zabo zikulu mulibe bantu; kulibe balibonse bapitamo. Vipangano vawanyika, mboni zasuliwa mutundu wabantu supasiwa ulemu. ***Volemba vakudala vachi Hebeli. vili na mau ya muzinda, koma ichi chiwonewa munga cho-onongewa kuli bolembewa bambili munga mau achi Hebeli mboni, ndiye kumasulila kwa ULB.*** ⁹ Ntaka ilila naku yuma; Lebanoni amvela nsoni naku yuma; ***liwu lakuti kulila linga belengeka munga kuyuma, Aba mau yabili ya chitebeli yalembewa chimozi mozi. Yesaya 24:4 yapalana, natanatuzo ija ionesa bwin kuyuma. Sharoni ali malo monha chipululu; ndipo Bashani na Carmel apulula matepu yabo. ¹⁰ "Manje niza nyemba, äkamba Yehova; "manje niza nyamuliwa pamwamba; mwaicho nizakwezekewa. ¹¹ Muli na mimba ya mauzu yoyuma mwa bala mapesi; kupema kwanu kuli munga mulilo wamene uzaku shokani imwe. ¹² Bantu baza shokew kunkala milota, munga vimitengo vaminga vimaduliwa naku shokewa. ¹³ Imwe bali kutali, mvelani vamene nachita; ndipo, imwe muli pafupi, zibani ukulu wanga." ¹⁴ Bochimwa mu Zayoni bali namanta; kunjenjema kwabagwila ba, ene balibe Mulungu. Niba ndani pakati banga yende paulendo na mulilo wokupya? Niba ndani pakati paife onga yende paulendo na mulilo wamuyayaya? ¹⁵ Uyo wamene ayenda moyela okukamba vazo-ona; Bamene sibakamaba pindu yaku dyakilila, bamene bamakunkumula manja yabo, Bamene ba vala matu yabo kuchoka ku kukesha manzi ndipo bamene bavala menso yabo kuti bsaone voipa- ¹⁶ Uyu ndiye muntu azakala pa mwamba, malo yake yochingiliwiza akankala nyumba yochingiliziwa pama lupili, vukdya vizakapiswa, na manzi yake siyaza kaymaba kusila. ¹⁷ Menso yabo yazakona mfumu mu ubwino wake; Bazaka onela malo patali. ¹⁸ Mutima wanu uzakumbuka choyofya; alikuti wamnene enzo lemba, bali kuti benzo pima ndalama? balikuti bamene benzo belenga ma tawa? ¹⁹ Simuzakaonapo futi bant bolakwa, chitundu chachi lend chamene simumunvela. ²⁰ Onani ku Zayoni, muzinda wama pwando yatu; menso yanu yazaona Yelusalemu malo yalibe chongo yankalamo, itema yamene siza kachosewa, vomangila vake siviza nyuliwapo olo chili chonse cha ntambo yake sichiza pwanyiwa. ²¹ Mumalo mwake, Yehova mu ulemelelo azankala naise, pa malo ya mimana ikulu kulibe bwato yonse yankondo ikulu iza endamo. ²² Pakuti Yehova ndiye woweluza watu Yehova ndiye ati pasa lamulo, Yehova ndiye mfumu; yatu azati pulumusa ife. ²³ Ma pila yanu siya manga; siyanga kwanise kugwililila hema mumalo yake; ndip sibaza kwanisa kuyanzika nyula yo yenzela chombo; pamene vo-onogeka vambili vagabanika nabo lemala baza tengako pavo onogeka. ²⁴ Bonkalamo sibaza kamba kuti, "ndine odwala;" bantu bamene ba nkala kuja sibaza kakulukiliwa ma chimo yabo.

Chapter 34

¹ Yandikirani, amitundu inu, mumve; tamverani, anthu inu! Dziko lapansi ndi zonse zili mmenemo ziyenera kumvera, dziko lapansi ndi zinthu zonse zochokera mmenemo. ² Pakuti Yehova wakwiyira amitundu onse, ndipo akwiyira magulu awo onse ankhondo; wawawonongeratu, wawapereka kukaphedwa. ³ Mitembo ya akufa awo idzaponyedwa kunja. Kununkha kwa mitembo kudzakhala paliponse; ndipo mapiri adzakhetsa magazi awo. ⁴ Nyenyezi zonse zakumwamba zidzatha, ndipo thambo lidzakulungidwa ngati mpukutu; ndipo nyenyezi zawo zonse zidzakomoka, monga tsamba lothothoka pa mpesa, ndi nkhuu zofesa pa mkuyu. ⁵ Pakuti pamene lupanga langa lidzamwe madzi kumwamba; taona tsopano udzagwera pa Edomu, pa anthu amene ndawapatula kuti awonongeke. ⁶ Lupanga la Yehova likukha magazi ndipo ladzazidwa ndi mafuta, magazi a ana a nkhusa ndi mbuzi, okutidwa ndi mafuta a impso za nkhusa zamphongo. Pakuti Yehova ali ndi nsembe ku Bozira, ndi kupha kwakukuru m'dziko la Edomu. ⁷ Ng'ombe zamtchire zidzagwa nazo, ndi ng'ombe zamphongo pamodzi ndi akulu. Dziko lawo lidzaledzera ndi magazi, ndi fumbi lawo lidzakhuta ndi mafuta. ⁸ Pakuti lidzakhala tsiku lobwezera Yehova, ndi chaka cha kubwezera chifukwa cha Ziyoni. ⁹ Mitsinje ya Edomu idzasanduka phula, ndi fumbi lake kukhala sulfure, ndi dziko lake lidzakhala phula loyaka moto. ¹⁰ Idzaotcha usiku ndi usana; utsi wake ukwera kosatha; lidzakhala labwinja m'mibadwo mibadwo; palibe amene adzadutsepo kunthawi za nthawi. ¹¹ Koma mbalame zamtchire ndi nyama zidzakhala mmenemo; kadzidzi ndi khwangwala adzapanga chisa chawo mmenemo. Adzatambasulirapo chingwe choyezera ndi chiwonongeko chakuwononga. ¹² Atsogoleri ake sadzasiyidwa ndi mawu oti ayitane ufumu, ndipo akalonga ake onse sadzakhala kanthu. ¹³ Minga idzadzaza nyumba zake zachifumu, lunguzi ndi mitula m'malo mwake; Udzakhala mokhalamo mimbulu, malo a nthiwatiwa. ¹⁴ Nyama zakutichire ndi afisi adzakumana kumeneko, ndipo mbuzi zamtchire zidzalira wina ndi mnzake. Nyama zakutichire zimakhazikika kumeneko ndikupeza malo ampumulo. ¹⁵ Ziwo bankhanga zimapanga zisa, kuikira mazira ndi kuwaswa, zimaswa ndi kuteteza ana awo. Inde, akamba azikasonkhana pamodzi, yense ndi mnzake. ¹⁶ Fufuzani mumpukutu wa Yehova; palibe imodzi mwa izi idzasowa. Palibe amene adzasowe wokwatirana naye; pakuti m'kamwa mwache adalamulira, ndipo mzimu wake udawasonkhanitsa. ¹⁷ Wachita maere kuti apeze malo awo, ndipo dzanja lake lawayeza ndi chingwe. Iwo adzakhala nazo mpaka kalekale. adzakhala kumeneko ku mibadwomibadwo.

Chapter 35

¹ Chipululu ndi Araba zidzakondwera; ndipo chipululu chidzakondwera ndi kuchita maluwa. Monga duwa, ² lidzaphuka mochuluka ndi kusangalala ndi chisangalalo ndi kuyimba; lidzapatsidwa ulemerero wa Lebano, ndi ukuru wa Karimeli ndi Sharoni; adzaona ulemerero wa Yehova, ndi ukulu wa Mulungu wathu; ³ Limbitsani manja ofooka, ndipo khazikitsani mawondo omwe agwedezeka. ⁴ Nenani kwa iwo a mitima yamantha, Limbani mtima, musaope; taonani, Mulungu wanu adza ndi kubwezera chilango, ndi mphoto ya Mulungu; adzabwera nadzakupulumutsani. ⁵ Pamenepo maso akhungu adzawona, ndi makutu a ogontha adzamva. ⁶ Pamenepo wopunduka adzatumphu ngati nswala, ndi lilime losalankhula lidzaimba; pakuti madzi atuluka m'Araba, ndi mitsinje m'chipululu. ⁷ Mchenga woyaka udzasandutsa dziwe, ndi nthaka youma idzakhala akasupe amadzi; m'malo a ankhandwe, momwemo zinakhalapo, padzakhala udzu ndi mabango ndi ubweya. ⁸ Kumeneko kudzakhala msewu waukulu wotchedwa Njira Yoyera. Wodetsedwa sadzayendamo. Koma zidzakhala za amene akuyenda momwemo. Palibe wopusa amene angachite izi. ⁹ Sipadzakhala mkango kumeneko, simudzakhala nyama yaukali; sadzapezeka kumeneko, koma owomboledwa adzayenda kumeneko. ¹⁰ Oomboledwa a Yehova adzabwera nadzafika ku Ziyoni akuyimba, ndi chimwemwe chosatha chidzakhala pa mitu yawo; kukondwa ndi chimwemwe zidzawapeza; chisoni ndi kuusa moyo kudzachoka.

Chapter 36

¹ M'chaka cha 14 cha Mfumu Hezekiya, Senakeribu mfumu ya Asuri anaukira mizinda yonse ya Yuda yokhala ndi mipanda yolimba kwambiri. ² Pamenepo mfumu ya Asuri inatumiza kazembe wamkulu wa nkondo kuchokera ku Lakisi kupita ku Yerusalemu kwa Mfumu Hezekiya ndi gulu lankhondo lalikulu. Adayandikira ngalande ya dziwe lakumtunda, panjira yayikulu yopita kumunda wa ochapa zovala, ndipo adayima pamenepo. ³ Aisraeli amene anatuluka mu mzindawo kukayankhula nawo anali Eliyakimu, mwana wa Hilikiya, woyang palaceanira nyumba yachifumu, Sebina mlembi wa mfumu, ndi Yowa mwana wa Asafu, amene analemba malamulo a boma. ⁴ Mkulu wa asilikaliyo anawawuza kuti, "Uzani Hezekiya kuti mfumu yayikulu, mfumu ya Asuri, yanena kuti, 'Kodi ukudalira chiyani?' ⁵ Mukungonena mawu opanda pake, kunena kuti pali uphungu ndi mphamvu zankhondo. wakhulupirira ndani wakupatsa iwe mphamvu kuti undiwukire? ⁶ Taona, ukukhulupirira ku Aigupto, bango lophwanyika lomwe umagwiritsa ntchito ngati ndodo yoyendamo, koma ngati munthu ayitsamira, limangirira m'manja mwake nalipyoza. Izi ndi zomwe Farao mfumu yaku Egypt ali kwa aliyense amene amamukhulupirira. ⁷ Koma mukadzanena kwa ine, Tikukhulupirira Yehova Mulungu wathu, kodi si iye amene Hezekiya wachotsa malo ake okwezeka ndi maguwa ake a nsembe, nati kwa Ayuda ndi kwa Yerusalemu, Mulambire pamaso pa guwa la nsembe ili ku Yerusalemu? " ⁸ Now therefore, I want to make you a good offer from my master the king of Assyria. I will give you two thousand horses, if you are able to find riders for them. ⁹ Kodi ungakane bwanji ngakhale kapitao mmodzi mwa akapolo aang'ono a mbuyanga? Wakhulupirira Igupto chifukwa cha magareta ndi apakavalo! ¹⁰ Tsopano, kodi ndapita kuno wopanda Yehova kukamenyana ndi dziko lino ndi kuliwononga? Pamenepo Yehova anandiuza kuti, 'Pita nawo m'dziko lino ndi kuliwononga.' " ¹¹ Pamenepo Eliyakimu mwana wa Hilikiya, ndi Sebina, ndi Yowa anati kwa kazembe wamkuluyo, Chonde lankhulani ndi anyamata anu m'Chiaramu, Chiaramu, chifukwa ife timachimva; musalankhule nafe m'chiyankhulo cha Ayuda, m'makutu athu; anthu amene ali pakhoma. " ¹² Koma mkulu wa asilikali anati, "Kodi mbuye wanga wandituma kwa mbuye wako ndi iwe kuti ndikayankhule mawu amenewa? ndi inu?" ¹³ Kenako mkulu wa asilikaliyo anaimirira ndi kufuula mokweza m'chilankhulo cha Chiyuda, kuti: "Tamverani mawu a mfumu yayikulu, mfumu ya Asuri. ¹⁴ Mfumuyo akuti, 'Musalole kuti Hezekiya akupusitseni, chifukwa sangakupulumutseni. ¹⁵ Musalole kuti Hezekiya akupangitseni kuti mudalire Yehova, ponena kuti, 'Yehova atipulumutsadi; mzinda uno sudzaperekedwa m'manja mwa mfumu ya Asuri. " ¹⁶ Musamvere Hezekiya, chifukwa mfumu ya Asuri yanena kuti, 'Pangani mgwirizano ndi ine, ndipo mubwere kwa ine. Pamenepo aliyense wa inu adzadya kuchokera ku mpesa wake ndi mkuyu wake, ndi kumwa madzi ake mu chitsime chake. ¹⁷ Mudzachita izi kufikira ndidzafika ndi kukutengerani ku dziko longa dziko lanu, dziko la tirigu ndi vinyo watsopano, dziko la mkate ndi minda yamphesa. ¹⁸ Musalole kuti Hezekiya akusocheretseni kuti, 'Yehova atipulumutsa.' Kodi milungu ya anthu a mitundu ina yawapulumutsa m'manja mwa mfumu ya Asuri? ¹⁹ Ili kuti milungu ya Hamati ndi Aripadi? Ili kuti milungu ya Sefaravaimu? Kodi analanditsa Samariya m'manja mwanga? ²⁰ Mwa milungu yonse yamayiko awa, kodi pali mulungu aliyense amene wapulumutsa dziko lake m'manja mwanga, ngati kuti Yehova adzapulumutsa Yerusalemu m'manja mwanga? " ²¹ Koma anthu adangokhala chete osayankha, popeza lamulo la mfumu lidati, "Musamuyankhe." ²² Pamenepo Eliyakimu mwana wa Hilikiya, woyang'anira nyumba yake, Sebina mlembi, ndi Yoa mwana wa Asafu wolembe mbiri, anadza kwa Hezekiya zovala zawo zitang'ambika, namuuza mawu a kazembe wamkulu.

Chapter 37

¹ Ndipo kunali, atamva mfumu Hezekiya, anang'amba zobvala zace, navala ciguduli, nalowa m'nyumba ya Yehova. ² Ndipo anatuma Eliyakimu, woyang'anira nyumba, ndi Sebina mlembi, ndi akulu a ansembe, onse atavala ziguduli, kwa mneneri Yesaya mwana wa Amози. ³ Nati kwa iye, Hezekiya anena, Lero ndilo tsiku losautsa, lodzudzula, ndi lotonza, monga ngati mwana ali pafupi kubadwa, koma amake alibe mphamvu yakubala mwana wao. ⁴ Kapena Mulungu wanu adzamva mawu a kazembe wamkulu, amene mbuye wake mfumu ya Asuri yamtuma kunyoza Mulungu wamoyo, nadzadzudzula mawu amene Yehova Mulungu wanu wamva. Tsopano kwezani pemphero lanu chifukwa cha otsala omwe alipo. ⁵ Pamenepo anyamata a Mfumu Hezekiya anadza kwa Yesaya, ⁶ nati kwa iwo, Nenani kwa mbuye wanu, Atero Yehova, Usaope mau amene wamva, amene anyamata a mfumu ya Asuri ananyoza nao; ine. ⁷ Taona ndidzaika mzimu mwa iye, ndipo adzamva mbiri yake, nadzabwerera kumka ku dziko lake. Ndidzamupha ndi lupanga m'dziko lake. ⁸ Pamenepo mkulu wa asilikali uja anabwerera ndipo anapeza mfumu ya Asuri ikumenyana ndi Libina, chifukwa inali itamva kuti mfumu yachoka ku Lakisi. ⁹ Pamenepo Sanakeribu anamva kuti Tirhaka mfumu ya Kusi ndi Aigupto apangana kuti amenyane naye; natumiza mithenga kwa Hezekiya, niti, ¹⁰ Nenani kwa Hezekiya, mfumu ya Yuda, Usanyenge Mulungu wako amene ukumkhulupirira; nati, Yerusalemu sadzaperekedwa m'manja a mfumu ya Asuri.

¹¹ Iwe wamva zimene mafumu a Asuri achita ku maiko onse powawonongeratu. Ndiye udzapulumutsidwa? ¹² Kodi milungu ya amitundu inawalanditsa, mitundu imene makolo anga anawononga: Gozani, Harana, ndi Rezefi, ndi anthu a ku Edene ku Tel Assar? ¹³ Ili kuti mfumu ya Hamati, mfumu ya Aripadi, mfumu ya midzi ya Sefaravaimu, Hena, ndi Iva? ¹⁴ Hezekiya analandira kalatayi kuchokera kwa amithenga ndipo anakawerenga. Kenako anapita kunyumba ya Yehova ndi kukaifungatira pamaso pake. ¹⁵ Hezekiya anapemphera kwa Yehova, nati, ¹⁶ "Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, inu amene mukhala pamwamba pa akerubi, Inu ndinu Mulungu wokha pa maufumu onse a dziko lapansi. Ndinu amene munapanga kumwamba ndi dziko lapansi. ¹⁷ Tcherani khutu lanu, Yehova, mumve. Tsegulani maso anu, Yehova, muwone, ndipo mverani mawu a Sanakeribu, amene watumiza kunyoza Mulungu wamoyo. ¹⁸ Ndizowona, Yehova, mafumu a Asuri awononga mitundu yonse ndi mayiko awo. ¹⁹ Aika milungu yawo pamoto, popeza sinali milungu koma ntchito ya manja a anthu, mitengo ndi miyala chabe. Choncho Asuri wawawononga. ²⁰ Tsopano, Yehova Mulungu wathu, mutipulumutse m'manja mwace, kuti maufumu onse a dziko lapansi adziwe kuti Inu ndinu Yehova, nokha. ²¹ Pamenepo Yesaya mwana wa Amози anatumiza kwa Hezekiya, kuti, Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, Popeza wandipempherera ine kwa Sanakeribu mfumu ya Asuri, ²² Yehova wayankhula za iye, namwaliyo a Ziyoni akunyoza ndi kukuseka akuseka; mwana wamkazi wa Yerusalemu akupukusa mutu chifukwa cha iwe. Ndi ndani amene iwe wamunyoza ndi kumchitira mwano? ²³ Kodi wakweza mawu ako ndi yani, ndipo unakweza maso ako pa kudzikuzi? Pamodzi ndi Woyera wa Isiraeli. ²⁴ Iwe wanyoza Yehova mwa akapolo ako, nati, Ndi magareta anga ambiri ndakwera pamwamba pa mapiri, pa zitunda zazitali za Lebano. Ndidzadula mitengo yake ya mkungudza italiitali ndi mitengo yamlombwa yabwino kwambiri, ndipo ndidzalowa m'itsmbali mwake, m'itsnkhhalango zake zobala zipatso kwambiri. Ine ndakumba zitsime ndi kumwa madzi; ²⁵ Ndidaumitsa mitsinje yonse ya Aigupto pansi pa mapazi anga. ²⁶ Kodi sunamve m'mene ndinatsimikiza mtima kale, ndi kuchigwiritsa ntchito masiku akale? Tsopano ndikubweretsa kuti zichitike. Muli pano kuti muchepetse mizinda yosagonjetseka kukhala milu yamabwinja. ²⁷ Anthu awo, opanda mphamvu, asweka ndi kuchita manyazi. Ndi mbewu zakumunda, udzu wobiriwira, udzu padenga kapena m'munda, mphepo yakum'mawa isanachitike. ²⁸ ²⁹ Koma ndikudziwa kukhala kwako pansi, kutuluka kwako, kulowa kwako, ndi mkwiyo wako pa ine. Chifukwa cha kundipsa mtima kwako, ndiponso chifukwa cha kudzikuzi kwako ndamva m'makutu mwanga, ndidzakunyamula ndi mbedza yanga m'kamwa mwako; Ndidzakubwezanso monga unadzera. ³⁰ Ichi chidzakhala chizindikiro kwa iwe: Chaka chino mudzadya zokolola zamtchire, ndipo chaka chachiwiri mudzadya zamtundu umenewo. Koma chaka chachitatu mudzale ndi kukolola, mudzalime minda yamphesa ndi kudya zipatso zake. ³¹ Otsala a nyumba ya Yuda amene adzapulumuke adzayambanso mizu ndi kubala zipatso. ³² Pakuti otsala adzaturuka m'Yerusalemu; opulumuka m'phiri la Ziyoni. Changu cha Yehova wa makamu chidzachita izi. ³³ Cifukwa cace Yehova atero za mfumu ya Asuri: "Sadzalowa mumzinda uno, kapena kuponyapo muvi kuno; sadza uyandikira ndi chishango, kapena kumangira linga iwo. ³⁴ adzakhala chimodzimodzi ndi momwe adzatulukire, ndipo sadzalowa m'mudzi uno; ati Yehova. ³⁵ Ndidzateteza mzinda uno ndi kuuwombola, chifukwa cha ine mwini, komanso chifukwa cha Davide mtumiki wanga. ³⁶ Kenako mngelo wa Yehova anapita kukamenya msasa wa Asuri, ndipo anapha asilikali 185,000. Anthuwo atadzuka m'mawa kwambiri, mitembo yogona inali paliponse. ³⁷ Natenepa Sanakeribu mambo wa Asirya abuluka ku Izraeli mbabwerera kunyumba mbakakhala ku Ninive. ³⁸ Pambuyo pake, atapembedza m

housenyumba ya mulungu wake Nisrok, ana ake aamuna Adrameleki ndi Sharezer anamupha ndi lupanga. Kenako anathawira kudziko la Ararati. Kenako Esarhaddon mwana wake anayamba kulamulira m'malo mwake.

Chapter 38

¹ Muma siku ya Hezekaya anadwala kufikila kuna kufa Chakuti Yesaya mwana waba Amosi, muneneli, anabwela kuli enve, anati, "Yehova akamba kuti, 'konani nyumba yanu bwino; ndaba muzafa, simuzankala na umoyo.'" ² Manje Hezekiya, nkope yake ana yangana pachi pupa nakupempela kuli Yehova. ³ Anakamba kuti, "Napapata, Yehova, nikumbukileni mwamene mwachikulupililo na pansi pamutima wanga nina yenda pamenso yanu." ⁴ Manje Hezekaya analila maningi nakupunda. ⁵ Ndipo mau ya Yehova yana bwela kuli Yesaya, kukamba kuti, "Yenda umuze Hezekaya, musogoleli wa bantu banga, "Ivi ndiye vamene Yehova, Mulungu wa Davide makolo banu, akamba kuti; namvela pempelo yako, ndipo naona misozi yako, yangona, niza lundako zaka 15 mu umoyo wako. ⁶ Ndipo niza kupulumusa na muzinda wako ku zanja ya mfumu yaku Asiliya, ndipo niza chingila uyu muzinda. ⁷ Ichi chizankala chiwonesela kuli imwe kuchokela kuli Yehova, kuti nizachita chamene ninaku uzani. ⁸ Yanganani, niza fendeza chinvwili nvwili pa ma stairs ya Ahazi kubwelela kumbuyo ma sitepu yali 10." Ndipo chinvwili nvwili chinafendela kumbuyo masitepu 10 pama stairs pamene chenye chinafika. ⁹ Iyi inali pemepelo yolembewa ya mfumu Hezekaya mfumu ya Yuda, pamene anali kudwala na pamene anapola: ¹⁰ "Ninakamnaba ivio nili pakati ka moyo wanga nizapitamo mumi lyango ya sheoli; natumiwa kumene kuja zaka zanga zonse. ¹¹ Nina kamba kuti siniza muona, Yehova mu chalo chaba moyo; Siniza bapepusa bantu bonse bonkala mu ziko lapansi***bantu bonse bonkala mu ziko lapansi: bena matembenezidwe asopano bali natantauzo iy. Ma kopi yakudala yaba Hebeli batantauza malo yamene bantu sibakalamo. (ndiye kuti mofupikisa munkalo)*** ¹² Umoyo wanga uzachosewa mwaine naku pelekewa monga musasa wa bobeta; na pomba umoyo wanga monga wo tunga; mwani chosamo motungila pakati ka siku na usiku mwa usilizai umoyo wanga. ¹³ Nina lila maningi ***liwu la chi Hebere ingabelengewe: Nina lila kapena nina zitontaza.***. kufikila kuseni; monga nkalamu apwanya yonse mafupa yanga. Pakati ka siku na usiku mwa usiliza umoyo wanga. ¹⁴ Manga imbiya nikuwaa; nikuwa monga njiba menso yanga yalema kuyangnila kumwamba, aAmbuye, nitadizeni. ¹⁵ Niza kamba chani? Ba kamba naine, ndipo bakwanisa; niza yenda pangano pagono zaka zonse pakui nagonjesewa nama dandaulo. ¹⁶ Ambuye, mavuto yamene mwatuma niya bwino kwa ine; nibwezeleli umoyo wanga kwa ine; mwani masulila umoyo na zau moyo zanga. ¹⁷ Chinali chokondwelesa kwa ine kupitamo mu madandaulo yabo mwani pulumusa mumu godi wa imfa; pakuti mwaponyela ma chimo yanga kumbuyo kwanu. ¹⁸ Na Sheol samayamikila iwe; imfa simamikila iwe; binse bamene bongena mumu godi balibe chikulupililo na chidalilo chanu. ¹⁹ Bantu bali na umoyo, nibamene batipsa zikomo, mwamene nachitila lelo; Batate bama onsesa ku bana ku daliliwa. ²⁰ Yehova afuna kuni pulumusa ine, ndipo tiza kondwela na nyimbo masiku yonse ya umoyo watu munyumba ya Yehova. ²¹ Manje Yesaya akamba kuti, "Lekani batenge mutolo wa mpesa naku zola pa chipute, ndipo aza pola." ²² Hezekaya naye ana kamba kuti, "kodi nichilangizo chiti chamene chizalangiza kuti niyendo ku nyumba ya Mulungu?"

Chapter 39

¹ Pantawi ija Marduk-baladani mwana wamwana wa balatani mfumu ya Babiloni, anatuma nkalata na mpaso kuli Hezekia; pamene ananvela kuti Hezekia anali wodwala ndipo apola. ² Hezekia anakondwela pali ivi vintu; analangiza botumikila bake munyumba yosungilamo vamutengo wodula- siliva, golide, tonunkula tumafuti tumafuta, nyumba yosungilamo zida za nkondo, na zonse zezikupezaka nyumba yake. Munalibe munyumba yake, kapena mu unfumu wake, chamene hwezekiah sanabalangize. ³ Pamene apo esaya anabwela kwa mfumu Hezekia namufunsa, "bushe aba bamuna bakamba chani kuli iwe? nanga bachokela kuti?" Hezekia anakamba kuti, "bachokela patali kuziko la babiloni." ⁴ Esaya anafunsa, " kodi baona chani munyumba yako?" Hezekia anayanka, "baonazonse munyumba yanga. Kulibe chamene sininabalangize chili munyumba yanga." ⁵ Esaya anakamba kuli Hezekia, "nvela mau a Yehova wamakamu: ⁶ 'Ona, masiku azabwela pamene vintu vonse vili munyumba ya mfumu, zintu zamene makolo anafaka kufikila siku yalelo, vizapelekewa ku babiloni. Kulibe chamene chizasala, akamba Yehova. ⁷ Bazatenga benangu bamumi bado yako, bamene azasunga, ndipo bazankala bolemekezeka munyumba ya mfumu wa Babiloni.'" ⁸ Ndipo Hezekia anakamba kuli Esaya, "mau ya Yehova yamene wakamba niyabwino." Chifukwa anaganiza monga, "kuzankala mutendele naku nkazikika mumasiku yanga."

Chapter 40

¹ "Limba, pantu bantu limbani," akamba mulungu wanu. ² "kambani na yerusalemu ; nakumuza kuti nkondo yasila, machimo yankululukidwa, nakuti alandila kabili kuchokela mumanja ya Yehova onse machimo ake." ³ Nvelani wina alila, "muchipulu kozani njila ya Yehova; pangilani mulungu njila yolondoloka mu Alabu." (enangu chungu chakudala amasula mau alila muchipulu monga mateyo 3:3") ⁴ Chigwa chilichonse chiza nyamuliwa, nama mapili na chulu yazalinganiziwa; ndipo malo yolimba yazalinganiziwa, ndipo malo ouma akhale chigwa; ⁵ na ulemelelo wa Yehova uzaoneka, ndipo bantu bonse bazauwona pamozi; chifukwa kamwa ya Yehova yakamba. ⁶ Mau yakamba, "lila." Winangu ayanka, "nanga nichani nilile?" "zamoyo zonse ni uzu, na zipangano zao zonse zokulupilika zili monga maluba ya muminda. ⁷ Mauzu yayuma na maluba ya fota Yehova akapemelako; zoonu umuntu nimauzu. ⁸ Mauzu yayuma, maluba yafota, koma mau ya mulungu watu yazankala kwamuyayaya." ⁹ Yenda pamwamba pa lupili, Ziyoni, iwe wamene uleta utenga wabwino. Punda maningi, Yerusalemu. Iwe wamene umaleta utenga wabwino, nyamula mau yako, usayope. Kamba kumizinda ya Yuda, "Uyu mulungu wanu!" ¹⁰ Ona, mulungu Yehova abwela monga owina wankondo, ndipo kwanja kwake kwa mpavwu kulumulila pa malo yake. Yangana, malipilo yake ali na eve, nabaja bamene apulumusa bayenda kusogolo kwake. ¹¹ Azakadyesa khosa zake monga woyanganila khosa, azafaka pamozi mu manja yake bana ba khosa, naku nyamula pafupi namutima wake, ndipo azazisogolela mbelele zamene zikulisa bana. ¹² Nindani wamene amapima manzi mumufolo yamanja yake, amapima na myamba na manja yake, amagwila fumbi ya ziko ya pansi mu basiketi, kupima mapili mu sikilo, kapena malundu olingana? ¹³ Nindani wamene amanvesa maganizo ya Yehova, kapena kumulangiza monga mlangizi? ¹⁴ Nikuchokela kuli ndani kwamene analandila chilangizo? Nindani anamupunzisa mochitila bwino vintu, naku mupunzisa nzelu, kapena kumulangiza njila yo nvesesa? ¹⁵ Ona, ma ziko ali monga donto yamu tsuko, ndipo yama oneka monga fumbi ilipa sikelo; amapima zilumba monga kadonto. ¹⁶ Lebanoni si mafuta yokwanila, kapena nyama zao nizokwanila kunkala nsembe zoshoka. ¹⁷ Maziko yonse siyokanila kuli eve; kuli eve yawoneka monga kulibe chiliko. ¹⁸ Nikulindani kwamene tingalinganize mulungu? Niku ka fano kati kwamene tinga mupalanise? ¹⁹ Kafano! bobaza bamataya; Bosula golide bamafaka golide pamwamba na kuipangila unyolo wa siliva. ²⁰ Kupanga nsembe umozi asanka mutengo wamene siuwola; asakila bamene baziba kubazakuti bapange fano yamene sizakagwa. ²¹ Mukalibe kuziba? Simunanvele? Sichinauziwe kuli imwe kuchokela kuchiyambi? Simunanvesese kuchokela pakuyamba kwa ziko ya pansi? ²² Niwamene amankala pamwamba patali maningi pa ziko yapansi; ndipo bonkalamo baoneka monga ziwala kuli eve. Amayodolola kumwamba monga nyula naku ya yanzika monga hema yonkalilamo. ²³ Amachefwa bolamulila kunkala bachabe nakupanga bolamulila bapa ziko ya pansi kankala balibe nchito. ²⁴ Amankala sioshangiriwa, osafesdwa, sinde zao sizinazike mizyu paziko ya pansi, akapemela pali zamene zimafoka, ndipo mpepo imazinyamula monga uzu. ²⁵ "Nikuli ndani kwamene munganilinganise, nindani wamene nipalana naye?" akamba woyera. ²⁶ Yangana kumwamba! Nindani analenga nyenyezi zonse izi? Amazosogolela monkalila nakuzi itana nazina. Kulinganiza na ukulu wa mpavwu zake ndipo na mpavwu za mpavwu zake, kulibe chosalila. ²⁷ Nichani mumakamba, Yakobo, naku lengeza, israeli, "njila yanga niyobisika kuli Yehova, ndipo mulungu wanga sayikila ko nzelu ku kusimikizila kwanga?" ²⁸ Nichani simuziba? Simunanvele? Mulungu wamuyayaya, Yehova, wamene analenga koyambila ziko ya pansi, samalema olo kufoka; kunvesesa kwake sikusila. ²⁹ Amapasa mpavwu kuli bolema; kuli bofoka amapasa mpanvu zanyowani. ³⁰ Muntu mung'ono aliyense amalema naku foka, ndipo ba muna bang'ono bama putwa naku kugwa: ³¹ koma bamene bama yembekezela pali Yehova azapanga mpavwu zao zanyowani; baza mbululuka namapapiko monga mpungu; bazakatamanga ndipo sibazaka foka; bazayenda ndipo sibaza komoka.

Chapter 41

¹ "Mvelani kuli ine osapanga chongo, lekani maziko yanklenso nampamvu; yabwele pafupi nakukamba tibwele pamozi nakusiliza ntota. ² Nindani wamene ayambanisa baku maba, kumu litana muchilungamo ku nchito yake? Apasila enve doti nalupanga wake, monga chimpepo chamene chi ulusa mapesi. ³ ba konaka nobapitilila, munjila mwamsanga kuti mendo yake yadyaka pangono pansi. ⁴ Nibandani ba chita ivi naku kwanilisa? nindani wamene ayitana mibadwa ku chokela ku chiyambi? Ine, Yehova, Oyamba, na osilizila, Ndine Ine. ⁵ Maziko yaku nyanja yaona yopa; kosilizila chalo kwa njema; Ba bwela. ⁶ Aliyense atandiza ba neba bake, na kukamba kuli wina na munzake, 'kulimbikisiwa.' ⁷ Mwaicho opala mapulanga alimbisa osula visulo golide, uyo osebenza na sando alimbisa osebenzesa chezulo, ku kamba voshokelela, nicabwino kokomela na misomali kuti chisagwe. ⁸ Koma, Isilayeli, banchito banga, Yakobo wamne nasanka, mubadwe Abrahamu munzanga, ⁹ Nina kutenngani ku chokela kumalile ya ziko yapansi nakuba itanani kuchokela kumali yakutali, kukamba kuli imwe, "Ndimwe ba nchito banga." Nakusankani imwe sinina kukaneni. ¹⁰ Musayope, pakuti nili naimwe, Musankale bamaganizo, pakuti ndine Mulungu wanu niza kulimbisani imwe, Nizakutandizani, ndipo nizakugwililani imwe nakwanja yanga ya manja yoyela. ¹¹ Onani, ba zamvela nsoni na manyazi, bonse bamene bali naukali kuli iwe; ba zankala bachabe chabe ndipo ba zaonongeka, abo bo sushana naimwe. ¹² Muzaka sakila simza kapeza abo boyamaba naimwe; abo bamene bachita nkondo naimwe azankala bachabe chabe, bosililato nchtio. ¹³ Chifukwa ine, Yehva Mulungu wanu, nizakagwilila kwanja yanu ya manja, kukamba kuli imwe, musayope, nikutandzani. ¹⁴ Musayope, Yakobo, iwe nyongololo, naimwe bamuna baku Isilayeli; niza kutandizani-nivamene akamba Yehova, okuwombolani wanu, oyela wa Isilayeli. ¹⁵ Onani, nikupangani imwe monga chisulo choshubilako, chanyowani na yonola-kubili imwe muzagaya malupili nakuya nyanyawula; muzapanga machul monga mauzu yoyuma. ¹⁶ muzaba kolola, ndipo mpepo iba nyamulila kutali; mpepo izaba mwazya. Muza kondwela muli Yehova, muza kondwela kulio oyela wa Isilayeli. ¹⁷ Bo dyakilila naba sauka bofuna manzi, koma kulibe, namalimi yabo yayuma nanjota; Ine, Yehova niza bayanka mapempelo yabo Ine, Mulungu wa Isilayeli, sinizabalekelela. ¹⁸ Niza panga mimana kutilila kumu tentemuko, na manzi yobils pakati pa vikwa. Nizalengea chipululu kunkala manzi, mumalo yoyuma manzi yobila. ¹⁹ Muchipululu nizaika keda, akesya, na mato, na mutengo wa olive. nizaika sipresi muchipululu, na pine na saipresi. ²⁰ Niza chita ichi kuti bantu ba one, bazindikile, bamvele pamozi, kuti kwanja kwa Yehova kwa chiya ivi, kuti oyela wa Isilayeli wazi panga. ²¹ "Letani mulandu wanu, "akamba Yehova, "Letani zamene mukambilako mafano yanu, "akamba mfumu ya Yakobo. ²² Lekani balete vosusha vawo kuli ise; babwele kusogolo bati uze vamene vizachitika, pakuti tivi ibe bwino. Ba tiuze vimene onakamba poyamba. kuti tikumbke naku ziba mwamen viza kwanilisiwa. ²³ Kambani vaku sogolo, kuti tizibe ngati ndimwe tumilungu; chitani vamushe olo voipa, kuti tiyope na kukondwla. ²⁴ Onani, Imwe mafano nimwe ba chabe chabe na vochita vanu; bamene baku sankani nibo kowela. ²⁵ Nanyamula umozi kuchokela ku mpoto, ndipo babwela; kuchokela pamene zuba ichoka ni itana bonse bamene baitana pa zina yanga, ndipo bazadyaka bolamulila monga matika, monga bobumba bamene badyaka doti yowumba. ²⁶ Niba ndani bana kamba ivi poyambilila, kuti tizibe? pambuyo pa ino ntawi, tingakambe kuti, "Bali bwino"? Nicho-ona palibe bamene bana chikamba, nizo-ona palibe anamvela kukamba kwanu. ²⁷ Nina kamba poyamba kuli Zayoni, "Onani aba bali apa:" Ninatumiza utenga ku Yelusalemu. ²⁸ Nikayangana, palibe bali bonse, palibe pali benve banga pase nzelu zabwino, bamene, nikaba funsa, banga yanke mau. ²⁹ Yangani, bonse balibe nchito, na zohia zabo zilibe nchito; na zisulo zabo na nsimbi zamangiwa zilibe nchito.

Chapter 42

¹ Taonani mtumiki wanga, amene ndimchirikiza; wosankhidwa wanga, mwa iye ndikondwera. Ndaika mzimu wanga pa iye; adzabweretsa chilungamo kwa amitundu. ² Sadzafuula kapena kufuula, kapena kumveka mawu ake m'misewu. ³ Bango lophwanyika sadzalithyola, ndi nyale yofuka sadzaizimitsa, adzachita chilungamo mokhulupirika. ⁴ Sadzalefuka kapena kutaya mtima kufikira atakhazikitsa chilungamo padziko lapansi; ndipo zilumba zidikira lamulo lake. ⁵ Atero Mulungu Yehova, amene analenga kumwamba, nawatambasula, amene analenga dziko lapansi ndi zonse za m'menemo, amene amapatsa anthu okhala mmenemo mpweya, ndi moyo kwa iwo akukhalamo: ⁶ Ine Yehova ndakuitana iwe m'chilungamo, ndipo ndidzagwira dzanja lako, ndidzakusunga ndi kukusunga ukhale pangano la anthu, ndi kuunika kwa amitundu, ⁷ kutsegula maso a akhungu, kumasula andende m'ndende, ndi m'nyumba yandende iwo akukhala mumdima. ⁸ Ine ndine Yehova; dzina langa ndi lomweli; ndipo ulemmerero wanga sindidzagawana ndi wina, kapena kunditamanda ndi mafano osemmedwa. ⁹ Onani, zinthu zam'mbuyomu zidakwaniritsidwa, tsopano ndatsala pang'ono kulengeza zochitika zatsopano. Zisanayambe kuchitika ndidzakuwuzani za izi. " ¹⁰ Imbirani Yehova nyimbo yatsopano, ndi matamando ake kuchokera kumalekezera a dziko lapansi; inu amene mutsikira kunyanja, ndi zonse zili mkati mwake, ndi zisumbu, ndi iwo akukhala momwemo. ¹¹ Chipululu ndi mizinda ifuule, midzi ya Kedara ayimbe; Okhala m'Sela ayimbe; afuule pamwamba pa mapiri. ¹² Alemekize Yehova, ndi kulengeza matamando ake m'zisumbu. ¹³ Yehova atuluka ngati wankhondo; ngati munthu wankhondo adzautsa nsanje yake. Adzafuula, inde, adzabangula phokoso la nkondo yake; adzaonetsa adani ake mphamvu zake. ¹⁴ Ndakhala chete kwa nthawi yayitali; Ndakhala chete ndipo ndinadziletsa; tsopano ndifuula ngati mkazi wobala; Ndipuma ndi kupuma. ¹⁵ Ndidzawononga mapiri ndi zitunda ndi kuimitsa msipu wawo wonse; ndipo ndidzasandutsa mitsinje zisumbu, ndi kuimitsa madambo. ¹⁶ Ndidzabweretsa akhungu m'njira imene sakudziwa; ndidzawatsogolera m'njira zimene sakudziwa. Ndidzasandutsa mdima kukhala kuunika pamaso pawo, ndi kukonza zopindika. Zinthu izi ndidzazichita, ndipo sindidzawasiya. ¹⁷ Adzabwerera m'mbuyo, nadzakhala ndi manyazi, iwo amene akhulupirira mafano osema, amene amati, "Inu ndinu milungu yathu." ¹⁸ Tamverani, agonthi inu; ndipo yang'anani inu akhungu, kuti muwone. ¹⁹ Ndani wakhungu koma wantchito wanga? Kapena wogontha ngati mthenga wanga amene ndimamutuma? Ndani ali wakhungu ngati mnzanga wapangano, kapena wakhungu ngati mtumiki wa Yahweh? ²⁰ Uwona zinthu zambiri, koma osazindikira; makutu ali otseguka, koma palibe amene akumva. ²¹ Zinakondweretsa Yehova kutamanda chilungamo chake ndi kupangitsa kuti malamulo ake akhale olemekizeka. ²² Koma awa ndi anthu olandidwa zofunkha; onse agwidwa m'maenje, ogwidwa m'ndende; akhala zofunkha popanda wowapulumsa, ndipo palibe amene akunena kuti, "Abweretseni!" ²³ Ndani mwa inu adzamvera izi? Ndani adzamve ndikumva mtsogolo? ²⁴ Ndani anapereka Yakobo kwa wolanda, ndi Israyeli kwa olanda? Kodi si Yehova, amene tidachimwira Iye, amene adakana kuyenda m'njira zake, ndi kukana kumvera lamulo lake? ²⁵ Cifukwa cace anatsanulira pa iwo mkwiyo wace waukuru ndi ciwawa ca nkondo; Malawi ao anawazinga, koma sanazindikira; chinawawotcha, koma sanachikumbukira.

Chapter 43

¹ Koma apa ichi nichamene Yehova akamba, wamene anakupanga, Yakobo, na wamene anakupanga iwe. Isilayeli; Usayope, chifuwa nina kuombolo iwe; nakuitana iwe pa zina yako, ndiwe wanga. ² Pamene upita mumanzi, nizankala naiwe; na kupiya kwa mu mimana, siizakutenga iwe. Pamene uzapita mu mulilo siuzapita, na chimbili mbili sichizakuononga. ³ Chifukwa ndine Yehova Mulungu wako, woyela eka wa Isilayeli, mupulumusi wabo. Nakipasa Igipito ngati malipilo, Kushi na Seba mukuchinjanisa naiwe. ⁴ Pakuti ndiwe wa mutengo wapata naku siyanako pamenso panga, nikukonda; mwaicho nizaika bantu pali iwe bochinjana na iwe, na bantu benangu bazangena mu moyo wake. ⁵ Usayope nili naiwe; Nizaleta bana bako kuchokela ku mawa, na kumi sonkanisani kuchoka ku mazulo. ⁶ Nizakamba ku mpoto, 'Bapelekeni kuli benve naku mwela, 'Osasiye aliwonse ku kumbuyo, 'Bwesani bana banga bamuna kuchoka kutali, na bana banga bakazi bochosa ku maziko ya kosizila ziko, ⁷ Aliwonse woitaniwa pa zina yanga, wamene nalenga pa ulemelelo wanga, Wamene ninaikapo, na wamene ni napanga. ⁸ Bachoseni bantu bamene sibaona, olo kuti bali namenso, na bosanvela, kapena bali ma matu. ⁹ Maiko yonse yakumana pamozi, na bantu bonse bosonkana. Wamene pakati pawo ngati anakamba ivo no kuzibisa kwa ife voyambilila vizachitika? Lekani babwelese umboni wayo kuti bazionesele kuti nichao-ona, balekeni banvele na kukamba, kuti, 'ni chazo-ona.' ¹⁰ Ndiwe mboni yanga, "Anakambilila Yehova, "na wanchito wanga wamene ninasanka, kuti iwe unga zibe na kukulupilila muli iwe, na kunvela kuti ndine wamene. Kumbuyo kwanga kunalibe Mulungu aliwonse, ndipo sikuzankala winanu kuchoka pali ine. ¹¹ Ine, Ndine Yehova, ndipo kulbe mupulumusi koma chaabe ine. ¹² Nina kambilila, kupulumuso, na kulalikila, ndipo sikuzonkala ka Mulungu pakati pa imwe. Ndiwe mboni yanga, akamba Yehova, ndine Mulungu. ¹³ Kuyambila lelo ndine wamene, ndipo kulibe wamene anga pulumuse aliwonse mu kwanja kwanga, Nima chita, ndipo nindani anga vibweze kumbuy?" ¹⁴ Ichi nichamene Yehva akamba, wokuombola, woyela wa Isilayeli: "Chifukwa cha iwe natumaku Babiloni na kubapeleka bonse kungsi monga botaba, kuchinja nyumba zochisangala za Babuloni mu nyimbo zolila. ¹⁵ Ndine Yehova, wako woyela, wamene analenga Isilayeli, mfumu yako." ¹⁶ Ivi nivamene Yehova akamba, wamene anasegula njila pa nyanja na njila mu manzi ya mpanvu. ¹⁷ Wamene anachosa galeta na kavala, yomenyayankondo na opambana. Bana gwela pasni pamozi; Sibazanyamuka nafuti; bazimiba, kuchosa monga chitnu chosilila choshokewa.) ¹⁸ "Osaganizila vintu vakudala, kapena ku kumbukila pa vintu vakudala. ¹⁹ Ona, nichiya chintu cha nyowani; apa manje chayamba kuchitika; siuchiona? Nizapanga njila muchipululu na misinje ya manzi muchipululu. ²⁰ Vinyama vamusanga viza nilemekeza, na magalu yamusanga na ntiba ntiba, chifkwa nimapasa manzi muchipululu, ma mimana muchipululu, kuti bantu banga bosankaiwa bakamwe, ²¹ aba bantu bamene nipanga baine neka, kuti banga kumbukile matamando yanga. ²² Koma simuna itane ine, Yacobo; mwalema naine, Isilayeli. ²³ Simunani bwelesele ine nkosa iliyonse ngati nsmebe yoshoka, kapena ku nipasa ulemu na zopeleka ahu zanseme. Sininakulemeseni imwe nazofunika zanseme. ²⁴ Siunanigulile ine zonunkila nzimbe iliyonse na ndalama, japena kuti unitaileko chiduswa chanyama yopeleka yako; koma wanilemesa ine namachimo yako, wani lemesa ine na vochitika vako voipa. ²⁵ Ine, nimwamene, Ine, wamene nimakuchosela volakwa vako vonse chifukwa cha zina yanga; ndipo sinizakumbuka machimo yako nafuti. ²⁶ Nikumbusa pali vamene vinachitka, leka tiganizile pamozi; bwelesa chifukwa chako kuti tione ngati uzapezeka ulibe mulandu. ²⁷ Batate bako boyamba banachimwa, naba sogoleli bako bamilakwila ine. ²⁸ Mwaicho nizaipisa boyangamila boyela; Nizamupeleka Yakobo muchionogeko chokwana, na Isialelyi kuti achite nsoni zovutisa."

Chapter 44

¹ Manje mvela, Yakobo wanchito wanga, na israeli wamene na sanku: ² ichi ndiye chamene Yehova akamba, eve wamene anakupanga nakuti lenga mu mimba na wamene azakundiza: "usayope, Yakobo wanchito wanga; naiwe Yeshurumu, wamene nasanka." ³ Pakuti niza tila manzi pa ntaka ya njota, na tumimana toyelela pa ntaka yoyuma; nizatila muzimu wanga pa bana bako na madaliso yanga pa mibado yako. ⁴ Baza mela pakati pa mauzu, monga matete yamene yapezeka mumbali mwamanzi. ⁵ Winango azakamba kuti, 'ndine wa Yehova,' na winango azaitana pa zina ya Yakobo, na winango azalemba pa kwanja pake 'wa Yehova,' nakupasa zina ati ndine israeli." ⁶ Ichi ndiye chamene Yehova akamba- mfumu ya israeli na muomboli wake Yehova wamakamu: "ndine woyamba, ndipo ndine wosiliza; elo kulibe mulungu koma ine." ⁷ Nindani alimonga ine? mulekeni akambe na kumasulila kuli ine vumene vana chitika kuchokela pamene nina nkazikisa bantubanga bakudala, futi mubasiye bakambe vumene vibwela kusogolo. ⁸ Musankala na manta nangu kuyopa. Sinina ku uzeni kudala, na kuchiwulula? Ndimwe akamboni banga: nanga kulipo mulungu kumbali kwa ine? kulibe mwala winangu; kulibe wumene niziba." ⁹ Bonse bamene bapanga tumilungu palibe mwamene balili; vintu vumene bakondwela navo niva chabe chabe; mboni zao sizinga one kapena kuziba chili chonse, ndipo baza nvesewa manyazi. ¹⁰ Nindani anga pange ka mulungu kapena kuka beza kamene kalibe nchito? ¹¹ Ona, bonse bamene agwilizana nabo baza nvesewa nsoni; bobaza ni bantu chabe. Lekani ba imilile pamozi; baza zionelamo na kunvesewa nsoni. ¹² Wosungunula vinsimbi amasebenza na vosebenzesa vake, kuvipanga, kusebenzesa malasha. Ama panga bwino bwino bwino na nsando nakusebenzesa kwanja yake ya mpavwu. Anvela njala, na mpavwu zake zayamba kusila, sa kumwa na manzi yali yonse nakubwela kukomoka. ¹³ Obaza amapima mitengo na ntambo, nakulembamo na cholembela. Amaipanga panga bwino na vosebenzesa vake na kulemba mizela na cholembela. Amaipanga kuoneka monga muntu, monga muntu wo oneka bwino, kuti chingankale munyumba. ¹⁴ Agwesa mitengo, kapena kusanka mitengo ya saipuresi kapena mtengo wa thundu. Amazisankila mitengo zikulu zikulu munsanga. Amashanga mitengo ndipo nvula ima ikulisa. ¹⁵ Ndipo muntu azusebenzesa kuyasha mulilo nakuzifundisa. Inde, ayasha mulilo nakupanga mukate. Nobwela kupangamo ka mulungu nakuka gwadila; ampanga fano naku igwadilila. ¹⁶ Ashokako mbali inango yachimutengo kuyashila mulilo, kushokelapo nyama yake. Akudya naku kuta. Azifundisa nakukamba kuti, "ah, nafunda, nauwona mulilo". ¹⁷ Mitengo zosalako apanga ka mulungu, fano yake yobaza; ayigwadila na kuyipasa ulemu, nakuyi pempela, "nipulumuse, pakuti ndiwe mulungu wanga," ¹⁸ Sibaziba, kapena kuzibisisa, pakuti menso yao niyakungu ndipo siyaona, na mitima zao sizinga zindikile. ¹⁹ Kulibe aganiza, kapena kunvesesa na kukamba, "nashoka mitengo zinangu mumulilo; inde, napanga futi mukate pa malasha yake. Nashoka nyama pa malasha yake na kudya. Manje nipange mbali inango ya nkuni kupanga chintu chinango chonyasa kuti nipembeze? ndiye kuti nigwade pansi kugwadila chiduswa chakuni?" ²⁰ Chili monga enze kudya milota; mutima wake wonamiwa unamusobesa. sangazipulumuse, kapena kukamba kuti, " ichi chintu chili mu kwanja yanga ya manja nika mulungu kaboza." ²¹ Ganiza pali ivi vintu, Yakobo, na israeli, pakuti ndiwe wanchito wanga: naku lenga; ndiwe wanchito wanga: israeli, suzakayibaliwa na ine. ²² Nachosapo, monga kumbi yo tikama, vochita vako vo ukila, ngati kumbi, machimo yako; bwelela kuli ine, pakuti nina kuombola. ²³ Imbani, imwe myamba, pakuti Yehova achita ivi , punda, iwe pansi pa ziko. Ngena chabe muku yimba, imwe mapili, na imwe sanga ya mitengo zo siyana siyana mukati; pakuti Yehova awombola Yakobo, na kulangiza ulemelelo wake mu israeli. ²⁴ Ivi ndiye vumene Yehova akamba, mu womboli wanu, wumene anakulenga mu mala: "ndine Yehova nina panga vonse, wumene eve eka ana tambasula myamba, wumene ana wamisa ziko ya pansi. ²⁵ Ine wumene nibweza kumbuyo bobwebweta bakamba vilibe nchito, na bamene ba sebanya bo belenga va obwebweta; ine wumene nina pindamula nzelu za bochenjela na kupanga malangizo yao kupusa. ²⁶ Ine, Yehova, wumene nina sikiza mau ya wanchito wake nakufikiliza mau yamene yanakambiwa na ntumi zake, wumene akamba pali yelusalemu, 'aza mkaliwamo , ' napa mizinda ya yuda, 'izamangiwa futi, ndipo nizamanga malo yo onongeka'; ²⁷ nindani wumene akamba ku nyanja yi tali, 'yuma, ndipo na tumimana twake tuza yuma.' ²⁸ Yehova ndiye akamba pali sailasi, 'ni mubusa wanga, wumene azachita chifuniro changa chonse; azakamba pali yelusalemu, 'azamangiwa futi,' na pa tempele, 'lekani maziko yake ya yikiwe.'"

Chapter 45

¹ Atero Yehova kwa wodzozedwa wake, kwa Koresi, amene ndagwira dzanja lake lamanja, kuti ndigonjetse mitundu pamaso pake, kulanda mafumu zida, ndi kutsegula zitseko pamaso pake, kuti zipata zikhale zotseguka: ² "Ndidzakutsogolera ndi kuyeza mapiri; ndidzathyola zitseko zamkuwa ndikuduladula mipiringidzo yawo yachitsulo, ³ ndipo ndidzakupatsa chuma cha mdima ndi chuma chobisika, kuti udziwe kuti ine ndine Inu Yehova, amene mumatchula dzina lanu, Ine ndine Mulungu wa Israyeli. ⁴ Chifukwa cha Yakobo mtumiki wanga, ndi Israyeli wosankhidwa wanga, ndakutchula dzina lako, ndakupatsa ulemu, ngakhale sunandidziwa. ⁵ Ine ndine Yehova, palibenso wina; palibenso Mulungu wina koma Ine ndekha. Ndikumangira nkondo, ngakhale sunandidziwe; ⁶ kuti anthu adziwe kuturukira dzuwa ndi kumadzulo, kuti palibe mulungu wina koma Ine; Ine ndine Yehova, ndipo palibenso wina. ⁷ Ndimapanga kuwala ndikupanga mdima; Ndimabweretsa mtendere ndi kubweretsa tsoka; Ine ndine Yehova, amene ndimachita zonsezi. ⁸ Inu kumwamba, mugwetse mvula kuchokera kumwamba! Thambo ligwetse chilungamo. Lolani kuti dziko lapansi lizame, kuti chipulumutso chikule, ndi chilungamo kuti chimere pamodzi nacho. Ine Yehova ndinazilenga zonsezi. ⁹ Tsoka kwa aliyense amene angatsutsane ndi amene adamupanga, iye amene ali ngati mphika uliwonse wa dothi pakati pa miphika yadothi ili yonse padziko lapansi! Kodi dongo limanena ndi woumba kuti, 'Mukupanga chiyani?' kapena 'Ntchito yanu ilibe choyang'anira?' ¹⁰ Tsoka kwa iye amene ati kwa atate wake, 'Mukulera chiyani?' kapena kwa mkazi, 'Ukala mwana uti?' ¹¹ Atero Yehova Woyera wa Israyeli, Mlengi wace, Ufunsiranji mafunso pazimene ndidzagitira ana anga? Kodi mundiuza choti ndichite ndi ntchito ya manja anga? ¹² 'Ndidapanga dziko lapansi ndikulengera munthu mmenemo. Anali manja anga amene anatambasula thambo, ndipo ndinalamula nyenyezi zonse kuti ziwonekere. ¹³ Ndinautsa Koresi m'chilungamo, ndipo ndidzasalaza njira zake zonse. Iye adzamanga mzinda wanga; adzalola anthu anga am'nsinga amuke kwawo, osati chifukwa cha mtengo waululu kapena ziphuphu, ati Yehova wa makamu. ¹⁴ Atero Yehova, Malipiro a Aigupto, ndi malonda a Kusi, pamodzi ndi Asabeya, amuna amsinkhu utali, adzabwera kwa iwe; kwa iwe ndikukuchonderera kuti, 'Zoonadi Mulungu ali ndi inu, ndipo palibenso wina kupatula iye. ¹⁵ "Zowonadi ndinu Mulungu amene amabisala, Mulungu wa Israeli, Mpulumutsi. ¹⁶ Onse adzachita manyazi ndi manyazi pamodzi; iwo osema mafano adzayenda monyozeka. ¹⁷ Koma Israyeli adzapulumutsidwa ndi Yehova ndi cipulumutso cosatha; sudzachitanso manyazi kapena kunyozeka. ¹⁸ Atero Yehova, amene adalenga kumwamba, Mulungu wona amene adalenga dziko lapansi, nalipanga, nalikhazikitsa. Adalilenga, osati ngati bwinja, koma adalikonzika kuti likhalemo: "Ine ndine Yehova, ndipo palibenso wina. ¹⁹ Sindinayankhule mseri, m'malo obisika; Sindinati kwa zidzukululu za Yakobo, 'Ndifuneni pachabe!' Ine ndine Yehova, amene ndinena zowona; Ndikulengeza zinthu zolondola. ²⁰ Sonkhanani ndipo bwerani! Sonkhanani pamodzi, inu othawa pakati pa amitundu! Alibe chidziwitso, iwo amene anyamula zifaniziro zogoba ndikupemphera kwa milungu yosakhoza kupulumutsa. ²¹ Bwerani pafupi mudzandidziwitse, bweretsani umboni! Aloleni iwo achite chiwembu pamodzi. Ndani waonetsa izi kalekale? Ndani adalengeza? Kodi sindine Yehova? Palibe Mulungu koma Ine, Mulungu wolungama, ndi Mpulumutsi; palibenso wina koma Ine ndekha. ²² Tembenukirani kwa ine ndi kupulumutsidwa, malekezere onse a dziko lapansi; pakuti Ine ndine Mulungu, ndipo palibenso wina. ²³ Ndikulumbira pa ine ndekha, ndikulankhula za chiweruzo changa, ndipo sichidzatembenuka: 'Ine ndidzapembedza mawondo onse, lirime lirilonse lidzalumbira. ²⁴ Adzanena za Ine, mwa Yehova mokha muli chipulumutso ndi mphamvu. ²⁵ Onse amene akumukwiwira adzachita manyazi. ²⁵ Mwa Yehova mbeu yonse ya Israyeli idzalungamitsidwa; adzadzitama mwa Iye.

Chapter 46

¹ Bel akuwerama, Nebo awerama. Mafano awo amalemera nyama zomwe amanyamula, ndipo inu mumakweza ng'ombe zanu ndi zolemetsa zakumwamba za nyama zotopa. ² Pamodzi amagwada pansi, agwada pansi; sangathe kupulumutsa zifanizo, ndipo iwonso atengedwa kupita ku ukapolo. ³ Mverani ine, nyumba ya Yakobo, otsala onse a nyumba ya Israyeli, amene ndanyamulidwa ndi inu ndisanabadwe, mudatulutsidwa m'mimba. ⁴ Ngakhale mpaka mudzakalambe Ine ndine, ndipo ngakhale tsitsi lanu laimvi ndidzakunyamulani. Ndinakupangani ndipo ndidzakusenzani; Ndidzakusenza ndipo ndidzakupulumutsa. ⁵ Mudzandifanizira ndi yani? Mukuganiza kuti ndifanana ndi ndani, kuti tifanane? ⁶ Anthu amatsanulira golide m'thumba ndipo amayesa siliva pasikelo. Amalemba ganyu wosula zitsulo, ndipo iye amapanga mulunguyo. amagwada nalambira. ⁷ Amanyamula pamapewa awo ndi kunyamula; amauika m'malo mwake, ndipo umayima m'malo mwake osasunthikapo. Amalira, koma sungayankhe kapena kupulumutsa aliyense ku mavuto ake. ⁸ Ganizani za izi; osawanyalanyaza, opanduka inu! ⁹ Ganizilani za zinthu zakale, za nthawi zakale: Ine ndine Mulungu, ndipo palibenso wina; Ine ndine Mulungu, ndipo palibenso wina wonga Ine. ¹⁰ Ndikulengeza chimaliziro kuyambira pachiyambi, ndi zisanachitike zomwe zisanachitike; Ndikuti, "Zolingalira zanga zichitika, ndipo ndichita momwe ndikufunira." ¹¹ Ndiyitana mbalame yolusa yakum'mawa, munthu amene ndinamusankha, kuchokera ku dziko lakutali; inde, ndanena; Ndidzachikwaniritsa; Ndatsimikiza mtima, ndipo ndidzachichitanso. ¹² Mverani Ine, anthu amitima yanu, amene mwachita zosalungama. ¹³ Ndikubweretsa chilungamo changa pafupi; sichiri patali, ndipo chipulumutso changa sichidikira; ndipo ndidzapulumutsa Ziyoni, ndi kukongola kwanga kwa Israyeli.

Chapter 47

¹ Tsika ukhale m'fumbi, namwaliwe, mwana wamkazi wa Babulo; khala pansi wopanda mpando wachifumu, mwana wamkazi wa Akasidi. Simudzatchedwanso ofooka komanso osakhwima. ² Tenga mphero, nupere ufa; chotsa chophimba chako, vula chovala chako chotseguka, vula miyendo yako, uwoloke mitsinje. ³ Umaliseche wako udzaululika, inde manyazi ako adzawoneka; ndidzabwezera, sindidzasunga munthu. ⁴ Wotiwoimbola, Yehova wa makamu dzina lake, Woyera wa Israyeli. ⁵ Khala chete, nulowe mumdima, mwana wamkazi wa Akasidi; chifukwa sudzatchedwanso mfumukazi ya maufumu. ⁶ Ndinakwiya ndi anthu anga; Ndinaipitsa colowa canga, ndipo ndinawapereka m'dzanja lanu, koma simunawacitira cifundo; munaika goli lolemera kwambiri pa anthu achikulire. ⁷ Inu munati, "Ndidzalamulira kwamuyaya monga mfumukazi yoyang'anira." Simudasamalire izi, ndipo simudaganizire za kukutulukirani. ⁸ Cifukwa cace tsono, imvani, okonda zokoma, khalani mosatekeseka; iwe amene unena mumtima mwako, Ndilipo, ndipo palibenso wina wonga Ine; sindidzakhala wamasiye, kapena kufedwa ana. ⁹ Koma zinthu ziwiri izi zidzakugwera m'kamphindi pa tsiku limodzi: kumwalira kwa ana ndi umasiye; adzakuthirirani mokwanira, ngakhale muli ndi nyanga, ndi mizimu, ndi zithumwa zambiri. ¹⁰ Wakhulupirira zoipa zako; wanena, Palibe wondiona ine; nzeru zako ndi chidziwitso chako zikusokeretsa iwe, koma iwe umanena mumtima mwako, "Ine ndilipo, ndipo palibenso wina wonga ine." ¹¹ Tsoka lidzakugonjetsa; simudzatha kuyithamangitsa ndi malingaliro anu. Chiwonongeko chidzakugwera; simudzatha kuzithamangitsa. Tsoka lidzakugwerani mwadzidzidzi, musanadziwe. ¹² Limbikirani kutaya matsenga anu ndi matsenga anu ambiri omwe mwawerenga mokhulupirika kuyambira muli mwana; mwina upambana, mwina ungawopsyeye tsoka. ¹³ Watopa ndi kufunsana kwako kochuluka; anthu amenewo ayimirire ndi kukupulumutsani — amene mulinganiza zakumwamba ndi kuyang'ana nyenyezi, amene munena za mwezi watsopano — asiyeni akupulumutseni ku zomwe zidzakuchitikireni. ¹⁴ Onani, adzakhala ngati mapesi. Moto udzawatentha. Sadzadzipulumutsa okha ku dzanja la moto. Kulibe makala amoto otenthetsera ndipo palibe moto woti akhalepo! ¹⁵ Izi ndi zimene akhala kwa iwe, amene ugwira nao nchito, amene wagula ndi kugulitsa nao kuyambira ubwana wako; anayenda yense m'njira yace; Palibe amene angakupulumutse. "

Chapter 48

¹ Imvani izi, inu a nyumba ya Yakobo, otchedwa ndi dzina loti Israeli, ndipo mwachokera ku umuna wa Yuda; inu amene mulumbira pa dzina la Yehova, ndi kupembedza Mulungu wa Israyeli, koma osati moona mtima kapena molongosoka. ² Chifukwa amadzitcha okha anthu a mzinda wopatulika ndipo amakhulupirira Mulungu wa Israeli. Yehova wa makamu ndiye dzina lake. ³ "Ine ndanena kale zinthu izi; zinatuluka m'kamwa mwanga, ndipo ndaziwitsa izo; ndipo mwadzidzidzi ndinazichita, ndipo zinachitika. ⁴ Popeza ndinadziwa kuti iwe uli wopulupudza, khosi lako lolimba ngati chitsulo, ndi chipumi chako ngati mkuwa, ⁵ chifukwa chake ndidayankhula izi kwa inu kale; zisanachitike ndidakuwuzani, kotero simunganene kuti, 'fano langa lazichita,' kapena 'Chithunzi changa chosema ndi chitsulo changa chosungika chakhazikitsa izi. . ' ⁶ Mudamva za izi; onani umboni wonsewu; ndipo inu, kodi simudzavomereza kuti zomwe ndanena ndizowona? Kuyambira tsopano, ndikuwonetsa zatsopano, zobisika zomwe simunadziwe. ⁷ Tsopano, osati kuyambira kale, zidakhalapo, ndipo lisanakhale lero sunamvepo za iwo, chifukwa chake sudzatha kunena, 'Inde, ndimadziwa za iwo.' ⁸ Simunamvepo; simunadziwe; izi sizinawululidwe kale. Pakuti ndinadziwa kuti ndiwe wonyenga kwambiri, ndi kuti wapanduka kuyambira ndili mwana. ⁹ Chifukwa cha dzina langa ndichedwetsa mkwiyo wanga, ndipo chifukwa cha ulemu wanga ndidzaletsa kukuwononga. ¹⁰ Taona ndinakuyenga koma osati ngati siliva; Ndakuyetsani m'ng'anjo yamasautso. ¹¹ Chifukwa cha Ine mwini, chifukwa cha Ine ndekha ndidzachita; Kodi ndingalole bwanji kuti dzina langa liipitsidwe? Sindidzapereka ulemu wanga kwa wina aliyense. ¹² Ndimvereni, Yakobo, ndi Israyeli, amene ndidamuyitana, Ndine; Ine ndine woyamba, ndipo inenso ndili womaliza. ¹³ Inde, dzanja langa linayala maziko a dziko lapansi, ndipo dzanja langa lamanja linayala kumwamba. ndikawaitana, aimirira pamodzi. ¹⁴ Sonkhanani pamodzi, nonse, kuti mumvetsere! Ndani mwa inu adalengeza zinthu izi? Mgwirizano wa Yahweh udzakwaniritsa cholinga chake chotsutsana ndi Babulo. Iye adzachita chifuniro cha Yehova pa Akasidi. ¹⁵ Ine, ndanena, ndamuyitana, ndabwera naye, ndipo apambana. ¹⁶ Yandikirani kwa ine, mverani ichi: Kuyambira pachiyambi sindinayankhula chobisika; zikachitika, ndidzakhala komweko. Tsopano Ambuye Yehova wandituma ine ndi Mzimu wake. ¹⁷ Atero Yehova, Mombolo wako, Woyera wa Israyeli, Ine ndine Yehova Mulungu wako, amene ndikuphunzitsa kuchita bwino, amene akukutsogolera ndi njira yoyenera kuyendamo, ¹⁸ ukadamvera malamulo anga; mtendere ndi chitukuko zikadayenda ngati mtsinje, ndi chipulumutso chako ngati mafunde a nyanja. ¹⁹ Atero Yehova, Mombolo wako, Woyera wa Israyeli, Ine ndine Yehova Mulungu wako, amene ndikuphunzitsa kuchita bwino, amene akukutsogolera ndi njira yoyenera kuyendamo, ukadamvera malamulo anga; mtendere ndi chitukuko zikadayenda ngati mtsinje, ndi chipulumutso chako ngati mafunde a nyanja. ²⁰ Tulukani ku Babulo! Thawirani kwa Akasidi! Ndi mawu akulira kufuulira! Dziwitsani izi, zipangeni kufikira malekezero adziko lapansi! Nenani, Yehova wawombola mtumiki wake Yakobo; ²¹ Iwo sanamve ludzu pamene iye anawatsogolera iwo kudutsa m'zipululu; adawatulutsira madzi thanthwe; anang'amba thanthwe, ndi madzi anaturuka. ²² Palibe mtendere kwa oipa, ati Yehova.

Chapter 49

¹ Nvela kuli ine, iwe kumbali kwa manzi! manje niveseni, imwe bantu bakutali. Yehova aniitana ine nazina yanga kuchokela pamene nina banda, pamene ba mayi banga bana ni bwelesa mu ziko. ² Anapanga kamwa kanga monga lupanga lakutwa, anani bisa ine muchiwili vwili cha manja ake; anani panga mivwi yo pangedwa bwino; mu mutuzi wake anibisa ine. ³ Anakamba kuli ine, "iwe ndiwe wanchito wanga, israeli, mwamene nilangiza ulemelelo wanga." ⁴ Koma nina yanka, "ngakale nina ganiza kuti nagwila nchito mwachabe, naononga mphavu yanga pa chabe, koma kuweluza kwanga kuli muli Yehova, namalipilo yanga ali kuli mulungu." ⁵ Manje Yehova anakamba -wamene ananiumba ine nikalibe ku badwa kuti mikankale wanchito wake, kubwezela Yakobo futi kuli eve kwakuti israeli akasokanisiwa kuli eve, chifukwa ndine wolemekezewa pa menso pa Yehova, ndipo mulungu ankala mphavu yanga - ⁶ ndipo akamba, "nikuti kang'ono kuti iwe unkale wanchito wanga kuti ukazikise mutundu ya Yakobo, na kubwezela opulumuka a israeli. Niza ku panga nyali ya bantu ba mitundu kuti unkale chipulumuso changa paka kusilizila kwa ziko." ⁷ Ichi ndiye chamene Yehova akamba, muomboli wa israeli, woyela wao, kuli uyo wamene umoyo wake niwo sulwi, ku zondewa na maiko, ndipo kapolo wa olamulila, "mafumu azakuonani nakunyamuka, na bana bafumu bazakuonani naku gwada pansi, chifukwa cha yehova wokulupilika, ngakale woyela wa israeli, wamene anakusanka iwe." ⁸ Ichi ndiye chamene Yehova akamba kuti, pa ntawi yamene naganizila kukulangiza chisomo niza kuyanka iwe, ndipo pa siku lachipulumusoniza kutandiza iwe; niza kuchingiliza iwe na kukupasa unkale pangano la bantu, kumanga malo, kubwezela malo osiwa malo olobelela. ⁹ Uzakamba kuli bomangidwa, 'chokani panja,' kuli abo bali mumigodi wofipa, 'zilangizeni inwe mweka.' Bazadyela mumbali mwamanjila, naku mutetemuka kulibe chilichonse kuzankala kodyela mauzu. ¹⁰ Sibazanvela njala olo njota; kapena kupya olo zuba sikuza fika pali beve, pakuti iye ali nachifundo pali beve azba sogolela beve; azabalangiza beve kumusinje ya manzi. ¹¹ Mwaicho niza panga mapili kunkala manjila, naku panga njila zitali kulinganiza." ¹² Onani, ichi chizabwela kuchokela kutali, vinangu kuchoka kumpoto na kumazulo; navinangu kuchoka ku malo a sinimu. ¹³ Imbani, kumwamba, na kusangala, ziko lapansi; mupwanyike mumaimbidwa, imwe mapili! pakuti Yehova atotoza bantu bake ndipo amanvela chisoni kuli bovutisiwa. ¹⁴ Koma ziyoni anakamba kuti, "Yehova anisiya ine ndipo ambuye aniibala ine," ¹⁵ "Kodi muyi angayibale mwana wake, amene anyonka, osanvela chisoni kuli mwana wamene anabala eka? Inde, bangaibale, koma ine sinizakuibala iwe." ¹⁶ Onani, nakulemala zina yako pamanja yanga; vipupozako vili pasogolo panga. ¹⁷ Bana bako babwela moyendesa, abo bamene banali kukuonanga bayenda. ¹⁸ Yangana mozuguluka nakuona, bonse bakusokana ku bwela kuli iwe. Pamene nikali na moyo -uku ndiye kukambila kwa Yehova - uzaba vala aba monga mabanga na kubafaka aba monga mukazi wofuna kukwatiliwa. ¹⁹ Ngakale munali zinyalala nakuchepekela, malo amene anali wonongeka, apo manje muzankala bang'ono mu malo yonkalapo, na bamene bana kuongani bazankala kutali. ²⁰ Bana bobadwa ntawi yamalilo yanu bazakamba mukunvela kwanu, 'malo niya ng'ono kuli ise tipezeleni malo, kuti tinkale kuno.' ²¹ Ndipo uza zifunsa iwe weka, 'nindani wamene anibalila aba bana ine? ninali wofelewa ndipo ngomwa, wotengewa ukapolo na kupishiwa kuchikwati. Nindani abakulisaaba bana? Onani, nenzeninasiiwa neka nanga ichi chachoka kuti?'" ²² Ichi ndiye chamene ambuye Yehova akamba kuti, "onani, nizanyamula kwanja yanga ku maiko; niza nyamula ndembela yachilangizo kuli bantu. Bazabwelesa bana bako bamuna mumanja nakunyamula bana bakazi bako muma mpewa. ²³ Mafumu azankala abambo alelo ako, nabakazi bamafumu iwe na khope yoyangana pansi nakumyanguta kakungu kaku mendo kwako; ndipo uzaziba kuti ndine yehova; abo bamene bayembekeza pali ine sibaza vesewa manyazi." ²⁴ Nanga chuma chingatengewe kuchokela kuli musilikali, kapena ogwiliwa kumasuliwa kuchokela kumukali? ²⁵ Koma icho ndiye chamene Yehova akamba kuti, "inde, bakapolo bazatengewa kuchoka kuli musilikali, na chuma chizapulumusiwa; pakuti nizalimbana nabo badani banu na kupulumusa bana banu. ²⁶ Nizadyesa okupondelezani nama nyama zao; ndipo bazakolewa namagazi yaobeka, monga ngati amwa vinyu. Ndipo mitundu zonse zizaziba kuti ine, Yehova, ndine mupulumusi wako ndipo wauombola, wa mphavu wa Yakobo."

Chapter 50

¹ Ndiye vamen Yehova akamba, "chilikuti chikalata chosiyana chamene ninasiyana bamai bako? Nikulibati bokongola bamene ninakugulisa. Ona, unagulisiwa chifukwa cha machimo yako, ndi chifukwa cho pandukila, bamai bako bana pishiwa. ² Chifukwa nichanoi nibwele uko popeza kulibe alionse? nitana kulibe ayanka? bushe kwanja yanga iyifupi kuti ninga kulipilile? bushe mulibe mpavwu muli ine kukupulumusa? Ona, muzulu kwanga nimayumika mimana, nimapanga mimana monga chipululu; nsomba zao zimafa mulandu wakusoba manzi nakuwola. ³ Nimavulika mu mwamba nimudima; navuikila na chinyula." ⁴ Yehova mulungu ananitansa lilime monga muntu wamene ana mpuzisiwa, kuti nakamba mau yachilimbiso kuli ofoka; amaniusha ine kuseniseni; amausa matu yanga kunvela monga bopunzila. ⁵ Ambuye Yehova asegula matu yanga, ndipo sininapandula olo ninabwelela kumbuyo. ⁶ Ninapasa mbuyo kuli bonse bamanimenya, na kumbali kwapamenso kuli abo bamene badonsa ndevu zanga; sininazibi nkope yanga muma chitidswe yao ya nsoni nakutunya. ⁷ Pakuti mulungu Yehehova azanitandiza; mwaicho sindine osebanike; mwaicho napanga nkope yanga yokosesa, chifukwa nizaba kuti sizanvela nsoni. ⁸ Wamene azanichitila chilungamo ali pafupi. Nindani wamene azanishusha? Tiyezi tiyimilile nakuonana naye wamene apasa milandu? Siyani abwele pafupi naine. ⁹ Ona, mulungu Yehova azanitandiza. Nindani wamene azakamba milandu yanga? Ona, yonse yazajujuka monga chovala; muswa uzavidya. ¹⁰ Nindani pali imwe wamene ayopa Yehova? wamene amakonka mau ya kapolo wake? Wamene amayenda mumudima ukulu kulibe nyali? Achetekele muzina ya Yehova na kusamila pali mulungu. ¹¹ Ona, bonse imwe bamene banyamula nyali za mulilo, mwane uzikonza nazosanikila, yendani munyali ya mililo na chimbilimbili chamene wayasha. Ichi ndiye chamene mwalandila kuchokela kuli ine: Muzakagona mumalo mobaba.

Chapter 51

¹ Nvelani kuli ine, imwe bamene mufuna chilingamo, imwe bamene musakila Yehova: yanganani pa mwala wamene munachezuliwako na kumyala yamene muna lubiwako. ² Yanganani pali Abulahamu, tate wanu na kuli sarai, anakubalani; pakuti pamene enze eka eve eka, nina munitana. Nina mudalisa eve naku mupanga kunkala bambili. ³ Zooni, Yehova aza puzyika ziyoni, aza puzyika malo yake yonse yo onongeka; chipululu chake ana chipanga monga Edeni, na madambo yake yami chipululu mumbali mwachigwa cha mumana wa yodani monga munda wa yehova; chisangalalo na chimwemwe viza pezeka muli eve, kuonga zikomo, na mau yo yimba. ⁴ "Nkalani omvesesa kuli ine, bantu banga; nakunvela kuli ine, bantu banga! Pakuti niza peleka cho kamba, niza panga chazooni changa nyali kuma ziko. ⁵ Chilungamo changa chili pafupi; chi pulumuso changa chiza chokapo, kwanja yanga iza weluza maziko; ma ziko yapatali maningi yazani yembekeza; kwanja yanga baza iyembekeza mofunisisa. ⁶ Nyamula menso yako ku mitambo, kuyangana pansu pa ziko, pakuti kumwamba kuzasila monga chusi, ziko lapansi iza silila monga chovala, na bonkalamo bazafa monga mainzi. Koma chipulumuso changa chizapitiliza mpaka muyayaya, na chilungamo changa sichizakasiyapo kusebenza. ⁷ Nvelani kuli ine, imwe bamene muziba cha bwino, imwe bantu muli na lamulo mumitima yanu: osayapa manyozo yabantu, kapena kupwanyika mutima paku vutisani kwao. ⁸ Pakuti munswa uza badya monga chovala, na nyongololo zizabadya monga ntambo otungila; koma chilungamo changa chizankala chamjuyayaya, nachipulumuso changa ku mibado yonse." ⁹ Ukani, ukani, zivalikeni na mpavwu, kwanja ya Yehova. Ukani monga mumasiku yakudala, mibado ya ntawi za kudala. Sindiwe wamene una shanyaula Rahabu, iwe wamene una boola chilombo? ¹⁰ Nanga simunayumike nyanja, manzi yopezeka pansu patali, na kupanga pansu panyanja njila yopitamo bo wombolewa? ¹¹ Bo pulumusiwa ba Yehova bazabwelela na kubwelela ku ziyoni na kulila kwa chisangalalo na chimwemwe chamuyayaya pa mitu zao; na chimwemwe na chisangalalo chizayenda pasogolo pao, na kukwimyilila na kulila kuza taba. ¹² Ine, ndine wamene niku puzyikani. Nichifukwa cha chani muchita manta na bantu, nindani azafa, bana bamuna ba bantu bopangiwa monga mauzu? ¹³ Nichifukwa cha chani mwa yibala yehova mulengi wanu, wamene ana tambusula kumwamba na kuyanzika maziko ya ziko ya pansu? Muli mumanta ya pafupi pafupi masiku onse chifukwa cha kupya kwa ukali wa odyakilila ngati ofuna kuononga. Uli kuti ukali wa odyakilila? ¹⁴ Eve wamene ofinisisa, Yehova aza endesa kusiyilila; sazafa na kuyenda pansu mu mugodi, kapena kusoba mukate. ¹⁵ Pakuti ndine Yehova mulungu wako, wamene amanga nyanja kuti chimpepo chake chi ulume- yehova wa makumu ndiye zina yake. ¹⁶ Na ika mau yanga mukamwa mwanu, na kukuvinikilani mu chinfwile cha kwanja yanga, kuti ninga shange myamba, kuyanzika ma ziko ya ziko la pansu, na kukamba kuli ziyoni, 'ndimwe bantu banga.'" ¹⁷ Uka, Uka, nyamuka yelusalemu, iwe wamene una mwela mukwanja ya Yehova kuchoka mumbale ya ukali wake; iwe wamene wamwela mumbale nakupitiliza kumwa moyendelela mu kapu yo zezelekesa. ¹⁸ Pakati pa bana bamuna bonse bamene anabala palibe wo musogolela; pakati pa bana bamuna bonse bamene anabala palibe wo musogolela; pakati pa bana ba bamene ana kulisa palibe wo mugwililila kwanja. ¹⁹ Aya mavuto yabili yanakuchitakilani- nindani azila na iwe? - kusiyiwa na kuonongeka, na njala na panga. Nindaniaza kupuzyika? ("mau yakale mu chi hebeli na kutantauzila kwingu kwamanje kukamba ati, "nizaku puzyikani bwani"? kutantauzila kwambili kwalelo kuma lembulula mau aya nakukamba kuti, "nindaniazakupuzyika"? ²⁰ Bana bako bamuna bakomoka; bagona pali ponse pokonekela njila, monga insha ili mu kombe; nibozuzyiwa na ukali wa Yehova kuzuzuliwa kwa ukali wa mulungu wanu. ²¹ Koma manje mvela ichi, iwe wodyakililwa na okolema, koma osati okolema na moba. ²² Mbuye wanu Yehova, mulungu wanu, wamene apapatila mulandu wa bantu bake, akamba ivi, "ona, nalema kapu yozezeleka kuchoka mukwanja yako - mbale, yamene ni kapu ya ukali wanga - kuti usa imwepo futi. ²³ Niza ifaka mumanja yabo kuvutisa, abo bana kuza ati 'gona pansu, 'gona pansu, kuti tiyende pamwamba pako'; unapanga musana wako monga mochaila bola na futi monga njila yao yoyendapo."

Chapter 52

¹ Ukani, ukani, fakani mpavu zanu, Ziyoni; valani zovala zabwino, Yelusalema, muzinda woyela; sikazachita kuli abo sibanaduliwe olo osayela kungena muli iwe. ² Zinyang'anye kuchoka mufumbi; nyamuka naku nkala, Yelusalemu; chosa macheni mumukosi wako, kapolo, mwana wa Ziyoni. ³ Pakuti ichi ndiye chamene Yehova akamba, "munagulisiwa pa chabe, ndipo muzaombolewa kulibe ndalama." ⁴ Ichi ndiye chamene akamba mulungu Yehova, "kuchiyambi bantu banga banayenda pansi mukunkala mu egupito; ndipo Asiriya abavutisa palibe na mulandu. ⁵ Manje nichani chamene nilinacho apa- uku nikukamba kwa Yehova- kuona kuti bantu banga bachosewa palibe mulandu? Bamene balamulila pali beve babaseka-uku nikumba kwa Yehova- ndipo zina yanga litakaniwa mopilila masiku yonse. ⁶ Mwaicho bantu banga bazaziba zina yanga; bazakaziba musiku ija kuti ndine wamene akamba, "inde, ndine!" ⁷ Mwamene kuwamila pamalupili ndiye mwamene alili mapazi yabo baleta utenga wabwino, bamene bakambilila mtendere, bali na mau yabwino, bamene bakambilila chipulumuso, bamene bakamba kuli Ziyoni, "mulungu wako alamulila!" ⁸ Nvela, bakamalonda bako banyamula mau yao, pamozi bapunda chosangalala, chifukwa bazawona, menso yao onse, Yehova abwelela ku Ziyoni. ⁹ Yimbani pamozi mokodwela, imwe mabwinja ya Yerusalemu; pakuti Yehova atotonza bantu bake; aombola Yerusalema. ¹⁰ Yehova atambusula kwanja kwake koyera pa menso ya maziko yonse; ma ziko ya pansi yazakaona chipulumuso cha mulungu. ¹¹ Choka, choka, yenda panja kuja; isagwile cjili chonse chamene sichoyela; choka pakati pao; zizeleseni mweka, muza nyamulazotengela za Yehova. ¹² Chifukwa simuzayenda motamanga, kapena kuchoka motangwanika; chifukwa Yehova azayenda pasogolo panu; ndipo mulungu wa israeli musogoleli wanu. ¹³ Ona, wanchito wanga azachita vintu na nzelu; azankala pamwamba naku nyamuliwa, ndipo azalemekezewa. ¹⁴ Monga mwamene bambili bana miyopani- mawonekedwe yake anayipisidwa kuchila mwamuna aliyense, ndipo anasiya kuoneka monga muntu. ¹⁵ Mwamene chilili, wanchito wanga azamwazika pa ziko na mfumu azavala makamwa yao chifukwa cha eve. Pali chiya chamene sibana uziwe, bazaona, ndipo nachamene sibana nvele, baza kaziba.

Chapter 53

¹ Ndani adakhulupirira zomwe adamva kwa ife, ndipo mkono wa Yehova wavumbulukira yani? ² Pakuti iye anakula pamaso pa Yehova ngati kamwana kakang'ono, ndi ngati msatsi panthaka youma; analibe mawonekedwe odabwitsa kapena kukongola; titamuwona, kunalibe kukongola kotikopa. ³ Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu; Munthu wazisoni, ndi wodziwa zowawa. Monga munthu amene anthu amabisala nkhope zawo, ananyozedwa; ndipo tidamuona kuti ndi wopanda pake. ⁴ Koma ndithu iye wanyamula nthenda zathu nanyamula zisoni zathu; komabe tinaganiza kuti akulangidwa ndi Mulungu, akumenyedwa ndi Mulungu, ndi kuzunzidwa. ⁵ Koma anapyozedwa chifukwa cha zochita zathu zopanduka; anaphwanyidwa chifukwa cha machimo athu. Chilango cha mtendere wathu chinali pa iye, ndipo ndi mabala ake ife tachiritsidwa. ⁶ Tonse tasochera ngati nkhoa; tayenda yense m'njira yake, ndipo Yehova waika pa iye mphulupulu ya tonsefe. ⁷ Iye anaponderezedwa; koma pamene anadzichepetsa, sanatsegula pakamwa pake; ngati mwanawankhosa wopita kukaphedwa, ndi ngati nkhoa imene iri chete pamaso pa omusenga, momwemo sanatsegula pakamwa pake. ⁸ Mwa kukakamizidwa ndi chiweruzo adatengedwa. Ponena za mbadwo wake, ndani adaganiza kuti adachotsedwa mdziko la amoyo, kapena kuti adalangidwa chifukwa cha zolakwa za anthu anga? ⁹ Anayika manda ake ndi achifwambawo, ndi munthu wachuma muimfa yake, ngakhale sanachite chiwawa chilichonse, kapena pakamwa pake panalibe chinyengo. ¹⁰ Komabe chinali chifuniro cha Yehova kuti amupondereze ndi kumudwalitsa. Akapanga moyo wake kukhala nsembe yamachimo, adzawona ana ake, adzatalikitsa masiku ake, ndipo cholinga cha Yehova chidzakwaniritsidwa kudzera mwa iye. ¹¹ Pambuyo pamavuto amoyo wake, adzawona kuwala ndikukhutitsidwa ndi chidziwitso chake. Mtumiki wanga wolungama adzalungamitsa ambiri; adzasenza mphulupulu zao. ¹² Chifukwa chake ndidzampatsa gawo lake pakati pa khamu la anthu, ndipo adzagawana zofunkha ndi ambiri, chifukwa adadziwonetsera yekha ku imfa ndipo adawerengedwa pamodzi ndi olakwa. Anasenza tchimo la ambiri ndikupembedzera olakwa.

Chapter 54

¹ Yimbani, iwe mukazi wosabala, iwe ukalibe kubala; yimbani mosangalala nakulila maningi, iwe wamene ukalibe kunkalapo na nchito yobala. Chifukwa bana masiye nibambili kuchila bana ba kazi wokwatiliwa," akamba Yehova. ² Kulisani mateti yanu naku yazika nyula za mateti mopitilila, kulibe kusiya; talipisani ntambo yanu naku ilimbisa mumitengo. ³ Chifukwa muzakatambusula ku zanja la manja naku zanja lamanzere, ndipo mibadwo yanu izapambana maziko naku nkala nafuti mumizinda yosauka. ⁴ Musayope chifukwa simuzanvesewa nsoni, kapena kukumudwisidwa chifukwa simuzanvela manyanzi; muzakaibala nsoni zamuchinyamata na manyanzi yosiyiwa. ⁵ Pakuti mulengi wanu ni mwamuna wanu; Yehova wamakamu ni zina yake. Woyela wa israeli ni muwomboli wanu; iyitaniwa kuti mulungu wa ziko yonse. ⁶ Chifukwa Yehova amitana nafuti munga mukazi osiyiwa naku kalipa mumuzimu, munga mukazi wokwatiliwa akachili mufana naku kukaniwa," akamba mulungu.

⁷ Kwa ntawi ing'ono ninamisiyani, koma nachifundo chikulu nizamifakani pamozi. ⁸ Mukukalipa kukulu nina bisa nkope yanga kuli imwe kwa ntawi; koma nachipangano chamuyayaya chokulupilika nizankala nachifundo naimwe- akamba Yehova, wamene azamupulumusa. ⁹ Chifukwa ichi chili munga manzi ya Nowa kuli ine: mwamene ninalapilila kuti manzi ya Nowa siyazakapita pa ziko ya pansi nafuti, nimwamene nalapilila na apa kuti sinizakamikalipilako nafuti kapena kuminyoza. ¹⁰ Ngakale malupili yangagwe na malundu yanganyang'anye, koma chikondi changa cholimba sichiza kachoka kuli imwe, kapena chipangano cha mutendere sichiza nyang'anya- akamba Yehova, alinachifundo naimwe. ¹¹ Bovutisiwa, boyenda na mpepo chikulu naba salimbisiwa, onani, nizayika mayendedwe yanu ya myala mu mtengo wapatali, ndipo niza yanzika maziko yanu na safaresi. ¹² Niza panga pamwamba pako na myala ya rubi na pongenela niza ika myala yobeka, na chipupa chapanja myala yabwino.

¹³ Ndipo bana banu bonse bazakapunzisiwa na Yehova; ndipo mutendere wabana banu uzankala ukulu. ¹⁴ Muchilungamo muza kaimilila, muzakankala kutali nakuvutisiwa, chifukwa simuzakayopa; nakuchokela ku manta, chifukwa siyaza kabwela pafupi naimwe. ¹⁵ Yanganani, mgati aliyense ayamba mavuto, siyaza kachoka kuli ine; aliyense ayamba mavuto naimwe azakagwa mukuluza. ¹⁶ Ona, ninapanga bobaza, bamene bapanga malasha yokupya nakupanga zida ya nchito yake, ndipo nina lenga wopwanya kupwanya. ¹⁷ Kulibe zida zamene zapangiliwa imwe zamene zizakachikelela; ndipo muzakonyoza aliyense azakamunizila. Ichi ndiye cholowa cha banchito ba Yehova, ndipo kusimikizila kwao kuchoka kuli ine- uku nikukamba kwa Yehova."

Chapter 55

¹ Anakamba kuli ine, "mwana wa muntu, imilila!" ndipo nizakamba na iwe". ² Ndipo, pamene anakamba na ine, Muzimu unangena muli ine nakuniyimilika na mendo yanga, ndipo nina mumvela ninshi anikambisa. ³ kukamba kuti, "Iwe mwana wa muntu, nikutumiza kuli bana ba Isilaeli, kuli mitundu yopondoka yamene inani pondokela-ndipo beve na makolo yao banichimwila kufikila lelo. ⁴ Bana bao bali na mfeshi zoyuma mukosi na mitima yoyuma. nikutuma kuli beve, ndipo ukabawuze kuti, 'Yehova Mbuye Mukulu maningi, akamba ati.' ⁵ Penango bazamvela kapena sibazamvela. Beve ni nyumba yo pondoka, koma baza ziba kuti penze muneneli pakati pao. ⁶ Iwe, mwana wa muntu, usabayope kapena mau yao. Usayope, olo uli na mitungwu na minga, olo unkala na nkanila; Usayope mau yao, olo kunkala manta na mfeshi zao, pakuti beve ni nyumba yo pondoka. ⁷ Koma uzabawuza mau yanga, olo bamvele olo basamvele, chifukwa nibopondoka maningi. ⁸ Koma iwe, mwana wa muntu, mvela vamene nikamba kuli iwe. Usankale wo pondoka monga nyumba ija yo pondoka. Segula mulomo wako udye chamene nizakupasa!" ⁹ Pamene apo nina yangana, ndipo kwanja inanitambasulila; mwamene umo mwenze cholembewa. ¹⁰ Eve anachitambasula pamenso panga; panalembewa kumbuyo na kusogolo kwake, ndipo penze polembewa ma lilo, na kulila na soka.

Chapter 3

¹ Anakamba kuli ine, Wobadwa ndi munthu iwe, idya chimene wapeza; ² Chotero ndinatsegula pakamwa panga, ndipo iye anandidyetsa mpukutuwo. ³ Ndipo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, idya mimba yako, nukhudze mimba yako ndi mpukutu uwu ndakupatsa. Choncho ndinaudya ndipo m’kamwa mwanga unazuna ngati uchi. ¹⁴ Mzimu unandinyamula ndi kunditenga, ndipo ndinamuka ndi kuwawa mtima mu ukali wa mzimu wanga, pakuti dzanja la Yehova linali kundikakamira mwamphamvu. ¹⁵ Choncho ndinapita kwa ogwidwa ku Teli Abibu okhala m’mphepete mwa Ngalande ya Kebara, ndipo ndinakhala kumeneko kwa masiku 7 , ndipo ndinadabwa kwambiri.

Chapter 9

¹ Pamenepo analilila mukunvela kwanga na mau yonveka, nati, Lekani wolanganila akwele kumuzinda, aliyense na chisulo chake chakupaila mumanja yake. ² Manje onani! Bamuna bali sikisi banatuluka munjila ya pachipata yakutali yolangana kumpoto, aliyense ali na chisulo chake chopaila mumanja mwake. Pakati pawo panali munthu wovala bafuta, ndipo mumbali mwake munali zisulo za mulembi. Choncho banangena mukati na kuimilila kumbali kwa guwa lansembe lamukuwa. ³ Ndipo ulemelelo wa Mulungu wa Isiraeli unakwela kuchokela pa akerubi nakufika pakomo pa nyumba. Iye anaitana munthu wovala bafutayo yamene yanali na zisulo za mulembi mumbali mwake. ⁴ Yehova anamuuzza kuti: "Pita pakati pa muzinda, pakati pa Yerusalemu, ulembe chizibiso pamphumi pa banthu bamene balila na kuusa moyo chifukwa cha vonyansa vonse vamene vichitika pakati pa muzinda. ⁵ Ndiponso anakamba na benangu mumakutu mwanga, Pita mumuzi pambuyo pake na kupaya. Usalengese menso yako kunkala na chifundo, ndipo usalekelele aliyense. ⁶ Paya-bonongelatu-mukulu bonse, munyamata, namwali, bana bang'ono kapena bakazi. Koma usakonke aliyense wamene ali na chizibiso pamutu pake. Muyambile pa malo yanga yopatulika!", Mwaichi banayambila na bakuli bamene banali pasogolo pa nyumba. ⁷ Anabauza kuti, "Ipisani nyumba, na kuzulisa panja pake na banthu bakufa. Ndipo banayenda na kuononga muzinda. ⁸ Pamene banali kuononga muzinda, ninazipeza neka na kugwesa nkope yanga pansi na kulila na kuti, : "Ha, Ambuye Yehova, nanga muzabononga bosala bonse ba Isiraeli pakubasanulila ukali wanu pa Yerusalemu? ⁹ Anakamba kuli ine, Uchimo wa nyumba ya Israyeli na Yuda niyaikul kwambili. Ziko yazula na magari na muzinda wazula na zopotoka, chifukwa bakamba kuti, Yehova aibala ziko, Yehova saona; ¹⁰ Koma kuli ine, linso yanga siizayangana na chifundo, ndipo sinizabalekelela. Mumalo mwake nibwelesa zonse pamutu pawo. ¹¹ Onani! Munthu wovala bafuta wamene anali na zida za mulembi mumbali mwake anabwelela. Anaulusa na kuti, Nachita vonse vamene munanilamulila."

Chapter 13

¹ Nafuti, mau ya Yehova yana bwela kuli ine, kuti, ² "Mwana wa muntu, nenela za baneneli bamene banenela mu Israeli na ku kamba kuli baja bamene banenela ku chokela mu maganizo yabo, 'Nvela mau ya Yehova,' ³ Mulungu Yehova akamba ichi: Soka kuli ba neneli bopusa, bamene bakonka mzimu yabo beka, koma kulibe chamene banaona! ⁴ Israeli, baneneli bako bankala monga mimbulu muchipululu ⁵ Simunayende kumalo yopwanyika yozunguluka nyumba ya Israeli kuti muikonze, kuti musiye kumenyana nabo pa siku ya Yehova. ⁶ Bantu bana menso mpenya yonama ndipo muma nenela vaboza, bamene bakamba, "ivi naivi ndiye vamene anakamba Yehova. Yehova sanabatume, koma apangisa bantu kuyembekezela kuti utenga wabo uzakwanilisiwa. ⁷ simunankale na menso penya yaboza na ku punzilila va boza, imwe bamene mukamba, Ivi naive ndiyeve anakamba Yehova" pamene ine neka sini nakambe?" ⁸ Pamene apo Mulungu Yehova akamba kuti, 'Popeza munaona mensompenya yonama na ku kamba vonama, chifukwa chake ni ivi vo kamba va Mulungu Yehova pali imwe: ⁹ kwanja yanga izankala pa ba neneli boona mensompenya yonama nabaja bamene banenela vaboza. Sibazankala pa gulu ya bantu banga, kapena kulembewa mu mabuku ya nyumba ya Israeli; basayende ku malo ya Israeli. Kuli iwe uzaziba kuti ine ndine Mulungu Yehova! ¹⁰ Chifukwa cha ichi, na chifukwa chakuti basobesa bantu banga, nati: "Mtendere! pamene palibe mtendere, akumanga mpanda wopaka laimu. ¹¹ Nena kwa iwo opaka linga, izagwa; kuzankala mvula yampamvu, ndipo nizatumiza matalala kuti igwese, na mpepo yamkunto kuti igwese pansi. ¹² Onani, chipupa chiizagwa. Sibanaku uzeni benangu, "ilikuti laimu yamene munafakako?" ¹³ Chifukwa cha ichi Ambuye Yehova bakamba kuti, Niza leta chimpepo chikulu, ndipo pazankala msinje ya mvula mu ukali wanga; Matalala mu ukali wanga yazauwononga kotheratu. ¹⁴ Pakuti nizagwesa linga yamene muna vininkila na laimu, ndipo nizaigweselatu pansi, ndipo pwaniyilatu paka pansi poyambila. Chotelo izagwa, ndipo naimwe muzawonongewa pakati pa ivo zonse. Pamenepo uzaziba kuti ine ndine Yehova. ¹⁵ Pakuti nizawononga chipupa na baja bamene banalipaka laimu na ku kwiya kwanga. Niza kamba kuli iwe: "chipupa sichilipo, ngakale bantu bamene banalipaka laimu, ¹⁶ baneneli ba Israeli bamene bananenela va Yerusalemu, bamene banaona mensompenya ya mtendele chifukwa pali eve, koma palibe mtendele!- uku niku nenela kwa Mulungu Yehova." ¹⁷ Iwe, mwana wa muntu, yangana nfeshi yako pa bana bakazi bantu ba mtundu bako, bamene banenela mumaganizo mwabo, naku kubanenela zoipa. ¹⁸ Kamba, 'Mulungu Yehova akamba: 'Soka kuli bakazi bamene bamasoka masenga mumanja mwabo, bamene bamavala nyla zochingila pamitu pabo za ukulu ulionse, zamene amasaka bantu. Muzasaka bantu banga koma kupulumusa moyo wanu? ¹⁹ Munani tukana pakati pa bantu banga chifukwa cha balele wozaza manja na zinyenyiswa za mukate, kuti mupaye bantu bamene simufunika kupaya, na kusunga muyo ya bamene sibafunikila kupitiliza na umoyo, chifukwa cha maboza yanu ku bantu banga bamene banu kunvelani. ²⁰ Mwaicho Mulungu Yehova, akamba ichi: 'sini funa zama mankwala zamasenga zamene mwasebenzesa ku gwila miyoyo ya bantu monga nyoni. Inde nizabamgamba kuchoka mumanja yanu; na bantu bamene mwagwila monga nyoni nizabalekelela bayende momasuka. ²¹ Nizangamba zopimba zanu na kupulumusa bantu banga mumanja mwanu, kuti basankale boteyewa mumanja mwanu. Uzaziba kuti ndine Yehova. ²² Chifukwa munafokesa mutima ya muntu olungama na maboza, nangu sina mukalipise, chifukwa mumalimbikisa zochita za munthu woipa kuti asasiye njila yake kuti apulumuse moyo wake. ²³ Mwaicho simuzaonapo mansompenya yonama, kapena kupunzila ufwiti, pakuti nizapuluma bantu banga mumanja mwanu. Uzaziwa kuti ine ndine Yehova.

Chapter 16

¹ Ndiponso mau a Yehova yanabwela kwa ine, kuti, ² Mwana wa munthu, zibisa Yerusalemu pa zonyansa zake, ³ nakukamba kuti, 'Ambuye Yehova akamba kuli Yerusalemu: Kuyamba kwako na kubadwa kwako kunachitikila mu malo ya Kanani; batate aako banali baku Maamori, na bamai banali baku Muhiti. ⁴ Pa siku ya kubadwa kwako, bamai bako sibanakucheke mukombo, kapena kukuyelesa na manzi, kapena kukuzoleka na muchele, kapena kukuvinkila nsalu. ⁵ Palibe linso linakuchitila iwe chifundo kukuchitila olo chimozi cha ivi vinthu, kuti akuchitile iwe chifundo. Pa siku yamene unabadwa, na kunyansidwa na moyo wako, unatayidwa panja pa munda. ⁶ Koma ninapita pafupi naiwe, ndipo ninakuona ukunyuka mumagazi yako; ndipo ninakamba kuli iwe mu magazi yako, Nkala na umoyo!" Ninakamba kuli iwe mumagazi yako, "Nkala na Umoyo!" ⁷ Ninakupanga iwe kukula monga zomela mumunda. Unabalana nakunkala wamukulu, ndipo unankhala ngale ya ngale. Maziba yako yanankala yolimba, na sisi yako inakula, ngakhale kuti unali wamaliseche ndipo kulbe zovala kumendo. ⁸ Ninapita kuli iwe nafuti, ndipo ninakuona. Ona! ntawi yachikondi inabwela kuli iwe, ninatambasula mukango pali iwe na kuvinkila chintako chako. Pamene apo ninalumbili kuli iwe nakukubwelesa mu chipangano-uku ndiko kukamba kwa Aambuye Yehova-ndipo unankala wanga. ⁹ Ninakusambika na manzi na kupukuta magazi kuchoka pali iwe, nakukuzoza na mafuta. ¹⁰ Ndinakuvalika zopikiwa zovala, na nsapato zachikopa kumendo kwako; Ninakuvinkila na nsalu yabwino, nakukuvinkila na siluku. ¹¹ Mopitiliza ninakuvalika juweli, nakuikapo vibangili kumanja kwako, na cheni mumukhosi mwako. ¹² Ninakuika ndolo mumpuno mwako, na ndolo mumakutu yako, na korona wabwino pamutu pako. ¹³ Mwaichi unaoneka bwino na golide na siliva, ndi kuvala bafuta, na silika, na zovala zopikiwa; unadya unga wabwino, uchi, na mafuta, ndipo unali kuoneka bwino kwambili, ndipo unankhala mfumukazi. ¹⁴ Mbili yako inanveka kwa bamitundu chifukwa cha kuoneka bwino kwako, chifukwa unali wangwilo mu ukulu wamene ninakupasa- mwamene akambila Ambuye Yehova. ¹⁵ Koma unadalila mu kuoneka bwino kwako, na kuchita vinthu monga hule chifukwa cha mbili yako; unatila zochita zako za uhule pali aliyense wamene anapita kwako, kuti kuoneka bwino kwako kunkale kwake. ¹⁶ Ndipo unatenga zovala zako na kuzipangila nazo malo yokwezeka yooneka bwino, ndipo kwamene kuja unachita vinthu monga hule. Ichi sembe sichinachitike. Kapena chinthu monga ichi kunkalapo. ¹⁷ Unatenga majuweli yooneka bwino ya golide na siliva yamene ninakupasa, na kuzipangila vooneka monga bamuna, na kuchita navo monga hule angachite. ¹⁸ Unatenga vovala vako vopikiwapikiwa na kuzivininkila, na kuika mafuta yanga monga zonunkila pamenso yawo. ¹⁹ Buledi yanga ninakupasa yopangiwa na fulao yabwino, na mafuta, na uchi, kuti unkhale na fungo yonunkhila bwino, ichi ndiye chamene akamba Ambuye Yehova. ²⁰ Koma unatenga bana bako bamuna na bakazi, bamene unanibalia ine, nakubapeleka nsembe kwa zifanizilo kuti badyewe monga vakudya. Ushe vochita vako va uhule ninkani ing'ono? ²¹ Unapaya bana banga kulu mafano na kubaocha mumulilo. ²² Muzonyansa zako zonse na zochita zako zachigololo siunaganizile za masiku ya ufana wako, pamene unali wopanda zovala na pamene unalibe chilichonse pamene unali kuvunvulika mumagazi yako. ²³ Soka! Soka kwa iwe! Uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova, mwaichi, mukuwonjezela pa vonse ivi voipa, ²⁴ unazipangila chitunda na kuzipangia malo yapamwamba pamalo yonse yozibika. ²⁵ Unamanga malo yako yapamwamba pa mutu wa njila iliyonse nakupanga kuoneka bwino kwako uchiwelewele, nakutambasula mendo yako kuli aliyense wamene apita, nakuchulukisa machitidwe yako ya uhule. ²⁶ Wachita zachigololo monga hule nama Aigupto, bapafupi pako wonyansa, na iwe munachita vambili vichitidwe va uhule, kunikwiisa kuukali wanga. ²⁷ Ona! Nizakumenya na kwanja kwanga nakujuba kuvakudya vako. Nizapeleka umoyo wako kuli badani bako, bana bakazi baku Afilisti, bamene banachita manyazi na zonyansa zako. ²⁸ Wachita machitidwe ya uhule pamozi na Asuri chifukwa siunakhutile. Unachita monga hule ndipo siunakhutile futi. ²⁹ Unachitanso zachiwelewele zambili muziko ya bogulisa baku Kasidi, na pali ichi siunakutile. ³⁰ Nanga mutima wako niwofoka bwanji—Uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova—kuti uzachita vonse ivi vinthu, nchito za uhule zilibe manyazi? ³¹ Wamanga zitunda zako pa mwamba pa museu ulibonse na kuzimangila malo yapatali mumalo yonveka yaliyonse. Koma siunankhale monga hule chifukwa unanyoza kulandila malipilo. ³² Iwe mukazi wachigololo, umalandila balendo mumalo mwa mwamuna wako. ³³ Banthu bamapeleka malipilo kwa hule iliyonse, koma iwe umapeleka malipilo yako kwa mabwenzi yako yonse, nakubapasa chiphuphu kuti babwele kwa iwe kuchokela kulikonse chifukwa cha uhule wako. ³⁴ Chifukwa cake pali kusiyana pakati pa iwe na bakazi benangu. Palibe wamene amakulipila kuti unkhale hule. Ndiwe bosiyana kwambili. Munawapasa malipilo ndipo siunapasidwe chilichonse. ³⁵ Mwaichi, iwe hule, mvela mau ya Yehova. ³⁶ Ambuye Yehova akamba kuti, Chifukwa watila panja kukumbwila kwako, kubonesa chintako chako mu zinchito zako zacigololo na okondewa bako na yonse mafano yako yonse yonyansa, na chifukwa unabapasa mwazi wa bana bako, ³⁷ Ona, nizasonkhanisa bonse bokondewa bako bamene unakumana nawo, bonse bamene unakondapo na bonse bamene unazondapo, ndipo

nizabasonkanisa mosusana naiwe kumbali iliyonse. Nizalangiza chintako chako kuli beve kuti bakuone. ³⁸ Pakuti nizakulanga chifukwa cha uhule na kukesa magari, na kukubwelesa pakukesa magari muukali wanga na nsanje zanga. ³⁹ Nizakupeleka iwe mumanja mwawo kuti bagwese chipinda chako chapamwamba, na kugwesa misanje yako, nakukuvula zovala zako, nakupoka zokuonesa bwino zonse. Bazakusiya chintako ndipo alibe kanthu. ⁴⁰ Ndipo bazabwelesa gulu yabanthu mosusana naiwe na kukutema miyala na miyala, na kukujuba muviduswa na malupanga yawo. ⁴¹ Bazashoka nyumba zako, nakukulangiza pamenso yabakazi bambili; pakuti nizalesa uhule wako, ndipo siuzabwezapu maubwenzi yako. ⁴² Pamenepo nizakazikika mutima wanga pansi pa iwe na ukali wanga; mukwiyo wanga uzachoka kuli iwe, pakuti nizakhuta, ndipo sinizankala bokalipa nafuti. ⁴³ Chifukwa siunakumbukie masiku ya ufana wako, na kunipanga ine kugwedeza ukali wanga chifukwa cha ivi vonse vinthu, mwaichi, Ona! Ine wamene nizakubwelesa pansi pa puthu wako chilango pazamene wachita-uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova. Kodi siunabonjezele vigololo pa zonyansa zako zonse? ⁴⁴ Onani! Aliyense wamene akamba miyambo kupitila mwa imwe azakamba kuti, Monga mayi alili, mwamene umo ali mwana wake wamkazi.” ⁴⁵ Iwe ndiwe mwana wamukazi wa mayi wako, wamene amanyansidwa na mwamuna wake na bana bake, ndipo ndiwe mlongo wa alongo ako amene amanyansidwa na bamuna bawo, bana bawo, bamai bako banali Muhiti, na batate bako banali Mwaamori. ⁴⁶ Kalongosi mukulu wako anali waku Samariya na bana bake bakazi banali kukhala kumpoto, pamene mung’ono wako anali kukhala kumumwela kwa iwe, ndiko kuti, Sodomu na bana bake bakazi. ⁴⁷ Simunayenda munjila zawo zeka, na kutenga mankalidwe yawo na machitidwe yawo, koma munjila zanu zonse munali woipa kuchila beve. ⁴⁸ Monga nili naumoyo, Ambuye Yehova akamba, kalongosi wako Sodomu na mizi yake, sibanachite choipa chili chonse monga wachichita iwe na bana bako bakazi. ⁴⁹ Onani! Yamene iyi inali chimo ya kalongosi wako Sodomu, kuti iye anali wozikuza mu umoyo wake wozitukumula, wosasamala ndiponso wosaganizila kalikonse. Sanalimbise manja ya banthu osauka na wosoba. ⁵⁰ Anali bozikuza na kuchita zonyansa pamenso panga, ndipo nizabachosa monga waonela. ⁵¹ Samaliya sanachite ngankale yang’ono pamachimo yako; Wachita vambili vonyansa vinthu kuchila vamene banachita, ndipo walengesa bakalongosi bako kuoneka wolungama kuchila iwe chifukwa cha vonse vonyansa vinthu vamene wachita! ⁵² Ubale manyazi yako, chifukwa waonesa bwino bakalongosi wako. Chifukwa cha machimo yako, yamene unachita monyansa, walengesa ba kalongosi bako kuoneka woyela kuchila iwe. Mwaichi, nkala wamanyazi na na kubala manyazi yako, chifukwa waonesa bakalongosi bako kuoneka woyela. ⁵³ Pakuti nizabweza undende wabo, ogwidwa baku Sodomu na bana bake bakazi, na bogwidwa ba Samariya na bana bake bakazi; ndipo bogwidwa bake bazankala pakati pawo. ⁵⁴ Cifukwa cha izi muzachita manyazi; uzankhala na manyazi chifukwa cha zonse zamene unachita, ndipo muli iyi njila muzankala chitontozo kuli beve. ⁵⁵ mwaichi kalongosi wako Sodomu na bana bake bakazi bazankalanso mwamene banalili poyamba, ndipo Samariya na minzi yake yabakazi bazankalanso mumalo yawo yakudala. Ndipo iwe na bana bako bakazi muzabwelela mwamene munalili kudala. ⁵⁶ Sodomu kalongosi wako sanakambiwepo ngankale mukamwa kako mu masiku yamene unali kuzinvela, ⁵⁷ pamene zoipa zako zikalibe kuululika. Manje uli kunyozewa na bana bakazi ba Edomu na kuli bonse bana bakazi baku Afilisti womuzungulila- wonse abo wokuzungulila bakuonelamo. ⁵⁸ Uzalangiza manyazi yako na zonyansa za machitidwe yako!— uku ndiye kukamba kwa Yehovah! ⁵⁹ Akamba Ambuye Yehova, Nizakuchitila iwe choyenela, iwe wamene wapepusa kulumbila kwako na kupwanya chipangano. ⁶⁰ Koma ine nizakumbukila chipangano changa chamene ninachita na iwe mumasiku ya ufana wako, ndipo nizapangana nawe chipangano chamuyaya. ⁶¹ Pamenepo muzakumbukila njila zanu, na kuchita manyazi polandila mulongo wanu na bakalongosi banu; Nizapeleka kwa iwe ngati bana bakazi, koma osati chifukwa cha chipangano chake. ⁶² Ine wamene nizankazikisa chipangano changa na iwe, ndipo uzaziba kuti ndine Yehova. ⁶³ Chifukwa cha ivi vinthu, uzaitana vilivonse kunzeli zako na kunkala wamanyazi, ndipo siuzasegulapo kamwa kako nakukamba chifukwa cha nsoni, pamene nakukulululika pali vonse vamene wachita-uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova.”

Chapter 18

¹ Mau ya Yehova yanabwela kuli ine, kuti, ² Kodi mutanthauuza chani, imwe bamene mukuchula mwambi wamene wukamba za ziko ya Isiraeli, kuti, 'Atate bamadya mphesa yosasamila, ndipo mano ya bana yapangiwa yofupa' ? ³ Pali Ine wamoyo- , ichi ndiye chamene Ambuye Yehova akamba- sipazakalanso cifukwa chonena mwambi uwu mu Israyeli. ⁴ Onani! Moyo uliwonse ni wanga- umoyo wa atate na umoyo wa mwana , ni wanga! Umoyo wachimwa ndiye wamene uzafa! ⁵ Kodi tingakambe chani za muntu olungama na ochita chilungamo - ⁶ ngati eve sakudya pamwamba pamapili kapena kukweza menso yake ku mafano yonyansa ya nyumba ya Isiraeli, samagona na mukazi wamuzake wapafupi kapena nakugona na mukazi ali kumwezi , kodi ni muntu wolungama? ⁷ Kodi tingakambe chani za muntu wamene sapondelela aliyense, wamene amabweza nkongole kuli wamene anankongolako, na wamene samaba koma amapasa vokudya kuli bali na njala na kuvinikila bamene balibe vovala- kodi muntu uyu ni wolungama ? ⁸ Kodi tingakambe chani pa muntu wamene salipilisa kuchuluka pa ndalama zamene akongolesa koma samachita zoipa nakwanja yake? Amanenewa kuti amachita chilungamo nakunkhazikisa kukhulupilila pakati pa banthu. ⁹ Ngati muntu ayenda mumalamulo yanga na kusunga malamulo yanga kuti azichita zintu mokhulupilila, lonjezano ya muntu wolungama ni iyi: Azankhala na umoyo - ichi ndiye chamene Ambuye Yehova akamba. ¹⁰ Koma ngati ali na mwana mwamuna wandeo wamene akesa magari, nakuchita chimozi cha vinthu ivi vakambiwa, ¹¹ (ngankale tate wake sanachite chilichonse cha ivi vinthu). Amadya pamwamba pamapili ndipo amagona na mukazi wamuzake wapafupi, tingakambe chani pali uyu? ¹² Eve amapondelela bosauka na bosoba ; amaba ndipo samabweza chikole, amakwezeka menso yake ku mafano na kuchita vinthu vonyansa, ¹³ ndipo amakongolesa ndalama naku onjezelapola chokwela kwambili, kodi muntu wamene uyu azankala na umoyo? Zoonazakankhala na umoyo ! Ndipo magari yake yazankala pali uyu chifukwa achita vinthu vonyansa. ¹⁴ Koma onani ! Ngati pali muntu wamene abala mwana mwamuna, ndipo mwana wake aona machimo yonse yamene bambo wake anachita, ndipo nangu aona, samachita vintu vamene ivi. ¹⁵ Mwana wamene uyu sakudya pamwamba pamapili, sama kwezeka menso yake kumafano ya munyumba ya Isiraeli, ndipo samagona na mukazi wamuzake wapafupi, kodi nichani chamene chingakambiwe pali eve ? ¹⁶ Mwana wamene uyu sapondelela aliyense, kapena kutenga chikole, kapena kutenga vintu vakuba, koma amapasa vakudya vake kuli bali nanjala na kuvinikila bamene balibe vovala. ¹⁷ Mwana uyu sapondelela muntu aliyense kapena kutenga chowonjezela chakuchulukila, koma achita malemba yanga nakuyenda monga mwa malemba yanga; mwana wamene uyu sazafa chifukwa cha chimo ya batate bake: eve azankala na umoyo! ¹⁸ Batate bake, kupeza kuti banapondelela bena mwa chinyengo naku bela mubale wake, nakuchita voipa kuli bantu ba mutundu wake- onani, azafa muzolakwa zake. ¹⁹ Koma imwe mukuti, 'Chifukwa nichani mwana savutikila machimo ya batate bake? Pakuti mwana uyu achita chiweluzo na chilungamo nakusunga malemba yanga yonse ; amavichita. Azankala na umoyo ! ²⁰ Wamene achimwa, ndiye wamene azafa. Mwana sazavutikila machimo ya batate bake, ndipo batate sibazavutikila machimo ya mwana wao. Chilungamo cha ochita zolungama chizankhala pali mwine, na kuipa kwa zoyipa kuzankala pali eve mwine. ²¹ Koma woyipa akatembenuka kusiya machimo yake yonse yamene anachita, nakusunga malemba yanga yonse, kuchita Vintu volungama, azankala na umoyo ndipo sazafa. ²² Volakwa vonse vamene anachita sivilakumbukilila futi. Azankhala na umoyo na chilungamo chamene amachita. ²³ Kodi ndimakondwela kwambili pa imfa yaboyipa— ivi vakambiwa na Ambuye Yehova- osati chifukwa chosiya njila yake kuti ankale na umoyo? ²⁴ Koma olungama akatembenuka kuleka chilungamo chake nakuchita machimo na vonyansa monga vonse vonyansa oipa achita, azankala na umoyo kodi? Volungama Vonse vamene anachita sivilakumbukiliwa pamene anigulisa muku chenjela kwake. Choncho azafa mumachimo yamene anachita. ²⁵ Koma imwe mukamba kuti, Njila ya Yehova si yolungama !' Mvelani, nyumba ya Israyeli! Kodi njila zanga ni zopanda chilungamo? Kodi si njila zanu zosalungama? ²⁶ Muntu olungama akabwelela kuleka chilungamo chake, nakuchita chimo nakufa chifukwa chamachimo , azafa chifukwa cha machimo yamene achita. ²⁷ Koma oipa akatembenuka kuleka voipa vake anachita, nakuweluzo kwa bwino na chilungamo, azasunga umoyo wake. ²⁸ Pakuti aona nakutembenuka kusiya volakwa vonse vamene anachita. Azankhala na umoyo, ndipo sazafa. ²⁹ ³⁰ Koma nyumba ya Israyeli ikamba kuti, 'Njila ya Yehova si yolungama!' Kodi njila yanga ili yosalungama bwanji, nyumba ya Isiraeli? Njila zanu ni zosalungama. Mwaichi nizaweluzo aliyense mwa imwe monga mwa njila zake, nyumba ya Isiraeli! Ichi chakambiwa na Ambuye Yehova . Tembenukani nakusiya volakwa vanu vonse kuti visankale vokuvalizani kushushana naimwe. ³¹ Tayani yonse machimo yamene munachita; pangani mitima na muzimu yanu inkale yasopano,kodi nichani chamene muzafela, nyumba ya Israeli ? ³² Chifukwa sinima sangalala muli infa ya muntu wamene afa- izi Ambuye Yehovah akamba- tembenukani naku nkala na umoyo ! "

Chapter 26

¹ Choncho muchaka chakumi na chimozi, siku yoyamba ya mwezi uja, mau ya Yehova yanabwela kuli ine, kukamba ² “Mwana wa muntu, chifukwa Turo anena moshuhsana na Yerusalemu, ‘Eya, zipata za bantu zatyolewa! Ani pindamukila; nizakuta chifukwa aonongeka.’ ³ Chifukwa chake Mulungu Yehova, akamba ichi, ‘Onani! “Ine nitana naiwe, Turo, ndipo nizaimya mitundu yambili ya bantu kuti ikumenyane naiwe, monga mwamene nyanja imaumilizila mafunde yake. ⁴ Bazaononga vipupa va Turo na kugwesa nsanja zake. Niza pyanga kalukungu kake monga mwala ilibe kantu. ⁵ Azankala malo poyumisa masumbo pakati pa nyanja, popeza nanela, uyu ni Mulungu Yehova, ndipo azankala otengewa monga katundu yankondo maiko ya mitundu. ⁶ bana bake bakazi bamene bali mu munda azapaiwa na lupanga, ndipo bazaziba kuti ine ndine Yehova. ⁷ Ichi ndachemene Ambuye Yehova akamba: onani, kuchokela kumwela kuleta Nebukadineza mfumu ya ku Babiloni, mfumu ya mafumu, kuchokela Tyre, nama kavalo, na magaleta, nabo kwela pakavalo, na bantu bambili. ⁸ Azapaya bana bako ba kazi mu munda na bemba. Azakumangilani mpanda na kukumanga mpanda pa makoma yako, na kukuikila zishango. ⁹ Azaika mbelele zimuna zogumulila zipupa zako, nazo sebenzesa zake azaagwesa zomangiwa zitali zako. ¹⁰ Makavalo yake yazankala yambilil kuti kavuluvulu kabo kaza ku vininkila. vipupa vako vizanyanganya pamozi na ku venka kwa bapa kavalo, chikochikala, na magaleta. Akangena pazipata zako, azangena monga mwamene bantu bamangenela mumzinda vamene vipupa vake vagwesewa. ¹¹ Mendo ya makavalo yake yazadyakiwa misebu yako yonse. Azapaya bantu bako na lupanga, ndipo zoimilisa zako za miyala zamphamvu zizagwa pansi. ¹² Beve bazalanda chuma chako na kulanda malonda yako. Beve bazagwesa vipupa vako na kuononga nyumba zako zapamwamba. Azataya miyala zako, matabwa yako na zinyalala zako mu manzi. ¹³ Nizalesa chongo cha nyimbo zanu. Kunveka kwa azeze bako sikuzamveka na futi. ¹⁴ Nizakusandusa mwala iibe kantu, ndipo uzankhala malo yoyanika sumbo kuti yayume. Suzamangiwanso mpaka kalekale, pakuti ine Yehova Mbuye nakamba kuti: “Uku ndiye ku kambilila kwa Ambuye Yehova. ¹⁵ Ambuye Yehova akamba ichi kuli Turo, zisumbu sizanyang'anisiwa na kunveka wa kugwa kwako, na kubula ko chitiwa, pamene kupaiwa kuli pakati pako? ¹⁶ Pamene akalonga bonse ba m'nyanja azasika pamipando yabo yachifumu a kuvula vovala vawo vachifumu na kuvula vovala vawo vopikapika. bazazivalika vovala kunjenjemela, azankala pansi na kunjenjemela ntawi yonse, ndipo azadabwa chifukwa cha imwe. ¹⁷ Bazakuimbilani nyimbo ya malilo pali mzinda, monga ichi mzinda ozibika, mwamene ba muna bambili banayenda mu nyanja kunkala manje sibalipo! Bantu bamuzinda uja ukulu banala na mphamvu zambili pamene bana nkala, koma manje banakala pansi pa nyanja; bana yofya bantu bonse bonkala pa pafupi nabeve. ¹⁸ Manje magombe banjenjemela pa siku po kugwa kwako. Zisumbu za munyanja zichita mantha, chifukwa suli mumalo mwako. ^{19 20 21} Ambuye Yehova akamba ichi, Nikalengesa munzi wabwinja, monga minzi yosankalamo bantu, nikazausha mabwinja yamene yalimbana naiwe, na pamene manzi yambili yazakuvininkila, manje niza kuleta pansi pali bantu bantawi yaku dala monga bamene banangena mu mugodi; chifukwa nizalengesa unkale malo yapansi maningi, monga ngati mabwinja yakudala; Chifukwa cha vamene ivi simuzabwelela na kuimilila mu ziko ya umoyo. Nizaika soka pali iwe, simuzankalamo futi mpaka muyayaya. ndipo azakufuna funa, koma simuzapezeka mpaka muyayaya, uku niku kambilila kwa Ambuye Yehova.

Chapter 28

¹ Pamene apo Yehova anapitiriza kukamba na ine kuti: ² “Iwe mwana wa muntu, uza wolamulila waku Turo kuti, ‘Yehova, Ambuye Wamkulu maningi, akamba kuti, ‘Mutima wako ni wozikuza.nizankala pa mupando wa milungu pakati pa nyanja!’” olo ndiwe muntu osati mulungu, umalengesa mutima wako kunkala munga mutima wa mulungu, ³ umaziwona munga wanzelu kuchila Danieli. palibe chisinsi chamene chimakudabwisani chimakudabwitsan! ⁴ Mwazilemeresa na nzelu na luso, ndipo mwapeza golide na siliva mosungila chuma mwanu! ⁵ Na nzelu zikulu na malonda yako, wapakisa chuma chako, ndipo mutima wako uzikuza chifukwa chachuma chako. ⁶ Chhifukwa cha ichi, akamba Ambuye Yehova, chifukwa waona munga mutima wako niwa mulungu, ⁷ nizakuletelani ba lendo, boyofya ba mitundu inango. beve bazaleta malupanga yawo pa kuwama kwanzelu zako, ndipo baza yifya ulemelelo wako. ⁸ Beve baza kugwesela mu chimugodi, ndipo uzafa imfa ya bantu bamene ba mafela mu nyanja. ⁹ nanga uzakamba kuti,” Ine ndine mulungu pamenso pa muntu wopaya iwe? imwe ndimwe muntu osati mulungu, ndipo muzankala mumanja mwa bamene bakulasani. ¹⁰ Uzafa imfa ya wosaduliwa na kwanja ya balendo, pakuti ine nakamba kuti-vamene ivi ndiye vamene YEHOVA AMBUYE Mukulu maningi, akamba. ¹¹ Yehova anapitiliza kukamba naine kuti: ¹² “Iwe mwana wa muntu, imba nyimbo yolila ya mfumu yaku Turo, ndipo uyi wuze ati, ‘Yehova, Ambuye mukulu maningi, akamba kuti: “wenze cholangizilako chabwino, wozula nanzelu ndiponso woyendelela mukuwama. ¹³ wenze mu edeni, mumunda wa mulungu: unali m’Edene, m’munda wa Mulungu: rube, topazi, emarodi, kulusolite, onekisi, yasipi, safiro, nofeki, na беру, voyikamo vako na vopachika vako vinapangiwa na golide. siku yamene unalengewa kuti vina konzewa. ¹⁴ Ninakuyika pa lupili yopatulika ya Mulungu wazoonza munga kerubi wamene ninazozza kuti asunge bantu. Iwe wenze pakati pa myala yoyaka mulilo wamene unayendayenda. ¹⁵ Unankala wabwino maningi munjila zako kuyambila siku yamene unalengewa, mpaka kusalungama kunapezeka muli iwe. ¹⁶ Chifukwa cha malonda yako yambili unazusha ndi ndewo ndipo unachimwa. mwa icho niza kuchosa mu lupili ya mulungu wa zoonza, munga muntu wodesedwa, ndipo nina kuwononga, iwe kerubi woyanganila, nakukuchosa pakati pa myala ya mulilo. ¹⁷ Mutima wako unazimvela na kuwama kwako; waononga nzelu zako chifukwa cha ulemelelo wako. Ine nakugwesela ku ziko yapansi. Nakuyika pamenso pa mafumu kuti bakuone. ¹⁸ Chifukwa cha kupaka kwamachimo yako na malonda yako ya boza, wadesa malo yako yopatulika. chifukwa cha icho nachosa mulilo muli iwe; vizakuwonongani. Nizakusandusa milota paziko ya pansu pamenso pa bonse bo kuwona. ¹⁹ Bonse bamene benze kukuzibani pa mitundu ya bantu bazanjenjema chifukwa cha iwe; baza nkala na manta, ndipo siwuzakankalako futi mpaka muyayaya. ²⁰ Pamene apo mau ya Yehova yana bwela kuli ine, kuti, ²¹ Wobadwa na muntu iwe, yangana mfeshi yako pali Zidoni, nakunenela vomushusha. ²² Ukambe ati, ‘Yehova, Ambuye mukulu maningi, akamba ati: “onani! Nilimbana naye, Sidoni! Pakuti nizalemekezewa pakati pako kuti bantu bako bazibe kuti ine ndine Yehova pakuchita chilungamo muli iwe. Nizalangiziwa kuti ndine woyera muli imwe. ²³ Ndizatumiza matenda yoyofya muli iwe, na magari munjila yako, ndipo bopayiwa bazagwa pakati pako. Lupanga ikakuzungulilani, muzaziba kuti ine ndine Yehova. ²⁴ Pamene apo sipazankala futi mitungwi yolasa na minga yobaba pa nyumba ya Israyeli kuchokela kuli bonse bomuzungulila, bamene bamene benze banasula bantu bake, ndipo bazaziba kuti ndine AMBUYE YEHOVA!’ ²⁵ Akamba AMBUYE YEHOVA, Nikasonkanisa nyumba ya Israyeli pa bantu bamene bamwazikana pakati pawo, na pamene nizapatuliwa pakati pawo, kuti bamitundu bawone, ²⁶ pamene apo bazamanga nyumba zawo muziko yamene nizapasa yakobo mutumiki wanga. ndipo azankala mukati mwake kulibe manta, nakumanga manyumba, nakulima minda ya mpesa, na kunkala balibe manta pamene nizachita chilungamo pali bonse bamene babasula pozungulila ponse; mwa ichi bazaziba kuti ine ndine Yehova Mulungu wawo.”

Chapter 31

¹ Ndipo muchaka chakhumi na chimozi, mumwezi wachitatu, siku yoyamba ya mwezi wamene uyo, Yehova ananiuza kuti: ² “Mwana wa munthu, kamba kuli Farao, mfumu ya Iguputo, na kwa makamu ya banthu bomuzungulila, ‘Muukulu wanu, mulimonga ndani?’ ³ Onani! Asuri anali mukunguza wa ku Lebano na byonkala na nthambi zooneka bwino, zopasa mthunzi kunkhalango, utali wamutali, na nsonga zake. ⁴ Manzi yambili yanachitalimphisa; manzi yambili yanachikulisa. Mimana inayenda mozungulila malo yake, chifukwa mimana yake inafikila mitengo yonse ya mumunda. ⁵ Muutali wake unapipilila mitengo inangu yonse ya mumunda, na nthambi zake zinankala zambili; nthambi zake zinakula chifukwa cha manzi yambili pamene zinakula. ⁶ Nyoni zonse za mumulengalenga zinamanga visa panthambi zake, na zamoyo zonse za mumunda zinabala bana bake pansi pa masamba yake. Mitundu yonse yambili ya banthu inkakhala muchfwile chake. ⁷ pakuti unali bokongola mu ukulu wake, na utali wa nthambi zake, pakuti mizyu yake inali mumanzi ambili. ⁸ Mikunguza ya mumunda wa Mulungu siinalingane nayo. Palibe mwa mitengo yamulombwa yolingana na nthambi zake, na mutengo wakupalana siunalingane na nthambi zake. Panalibe mutengo wina mumunda wa Mulungu wolingana naiye mukukongola kwake, ⁹ ninaukongolesa na nthambi zake. nthambi zake zambili na zonse mitengo zamu Edene imene inali mumunda wa Mulungu inauchitila nsanje. ¹⁰ Mwaichi Ambuye Yehova akamba ichi: Chifukwa chinali chitali mu utali, nakugwililila utali pakati pa nthambi zake, unakweza mutima wake chifukwa cha utali wake; ¹¹ Naupeleka mumanja mwa munthu wamphamvu pakati pa bamitundu, kuti auchite molingana na kuipa kwake. Nazitaya. ¹² Balendo bamene banachititsa mantha maziko yonse banajuba na kuisiya kuti bafe. Nthambi zake zinagwela pamapili na muzigwa zonse, na nthambi zake zinathyoka muzigwa zonse za ziko. Ndipo maziko yonse ya banthu paziko yapansi inatuluka mumuthunzi wake ndipo inachokamo. ¹³ Mbalame zonse za mumulengalenga zinapumulila pa sinde ya mutengo wakugwa, na nyama zonse za mumunda zinabwela ntambi zake. ¹⁴ Izi zinachitika kuti mitengo inangu yonse imene imamela mumbali mwa manzi isadzakweze masamba ake mpaka kufika pamtunda wautali kwambili, ndiponso kuti pasakhalenso mitengo ina imene imamera m’mphepete mwa madziwo imene izafika msinkhu umenewu. Bonse awo banapelekewa ku imfa, pansi pa ziko lapansi, mwa bana ba banthu, pamozi na bonse oyenda pansi mumugodi. ¹⁵ Ambuye Yehova wakamba ichi: Pa siku yamene mutengo wa seda unayenda pansi, ninabwelesa chisoni paziko lapansi. Ninavininkila mazi yakuya pamwamba pake, na kugwilila manzi yamu nyanja. Ninagwililila manzi yamphavu, na kubwelesa chisoni ku Lebanoni chifukwa cha eve. Mwaichi yonse mitengo ya mumunda inalila chifukwa cha zamene izi. ¹⁶ Ninagwesa kunjenjemela kwa maziko pakumva chongo cha kugwa kwake, pamene ninauponya kumanda, pamozi na beve oselukila mumugodi. Mwaichi ninatontoza mitengo yonse yamu Edene muni mwa ziko lapansi. Iyi inali mitengo yosankhika na yabwino koposa ya ku Lebano; mitengo imene inamwa manzi. ¹⁷ Pakuti nabonso banayenda nabo pansi, kuli awo bamene banapaiwa na lupanga. Bamene awo banali manja yolimba, ayo maziko yamene yanankala muchfwile chake. ¹⁸ Ni mitengo iti ya mu Edeni inali yolingana na imwe mu ulemelelo na ukulu? Pakuti uzayenda pansi pamozi na mitengo ya Edeni ku malekezelo kwa ziko yapansi pakati pa banthu osadulidwa; uzankala na umoyo pamozi na beve bamene banapaiwa na lupanga.

Chapter 34

¹ Ndipo mau ya Yehova yanabwela kwa ine, kuti, ² Mwana wamunthu, nenela mosusana nama busa ba Israyeli. Nenela nakubauza kuti, 'Ambuye Yehova akamba izi kuli ba zibusa: 'Soka kuli abusa ba Isiraeli bamene bazitumikila beka. Kodi abusa sibafunika kuyanganila gulu la nkhusa?' ³ Mumadya zonona na kuvala za usako. Mumapaya zoina za zobeta. Simubeta kali konse. ⁴ Simunalimbikise awo bamene bali wofoka, kapena kuchilisa odwala. Simumanga bamene bali botyoka, ndipo simubweza zotamangisidwa, kapena kufunafuna zotayika. Mumalo mwake, mukubalamulila mwa mphanvu na mwachongo. ⁵ Ndipo banabalalika kulibe mubusa, ndipo banankala chakudya cha vilombo vonse va musanga, pambuyo pobalalika. ⁶ Nkhosa zanga zasobela pamapili yonse napa chulu chachitali, ndipo zabalalika paziko lonse lapansi. Koma palibe wamene azifuna. ⁷ Chifukwa chake, abusa, imvani mau ya Yehova: ⁸ nikali namoyo-uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova-, chifukwa zibeto zanga zсандuka zofunkha na chakudya cha zobeta zonse za musanga, chifukwa panalibe mubusa, ndipo palibe ba busa banga banafuna funa gulu yanga; ba busa banazisunga, wosabeta nkhusa zanga. ⁹ Chifukwa chake, abusa, imvani mau ya Yehova: ¹⁰ Ambuye Yehova bakamba: Taonani! Nisusana na azibusa, ndipo nizafuna nkhusa zanga mumanja mwawo. pamenepo nizabachosa asamawete zoweta; ndipo abusa sazazichepesanso, popeza nizachosa nkhusa zanga pakamwa pao, kuti zisankalenso chakudya chawo. ¹¹ Pakuti Ambuye Yehova akamba ichi: Taonani! Ine neka nizafunafuna nkosa zanga na kuzisamalila, ¹² monga mubusa wamene ali kufunafuna nkhusa zake siku yamene ali pakati pa gulu yake yobalalika. Mwaichi nizafunafuna nkhusa zanga, ndipo nizazipulumusa mumalo monse mumene zinabalalikila siku ya makumbi na mudima. ¹³ Pamenepo nizabatulusa pakati pa mitundu ya banthu; Nizabasonkanisa kuchokela mumaziko na kubabwelesa ku ziko yawo. Nizabaika mumalo odyeselako zibeto mumapili ya Isiraeli, mosilila mwa mimana, na mumenzi yonse ya muziko. ¹⁴ nizazifaka muli babusa babwino; mapili yatali ya Israyeli yazankhala malo yawo yodyeselako zibeto. Zizagona mumalo yabwino yodyeselako zibeto mumalo yodyeselako zobeta zambili, ndipo zizadya misipu mumapili ya Isiraeli. ¹⁵ Ine wamene nizabeta nkosa zanga, ndipo ine wamene nizazigonesa nekha-ichi ndiye chamene Ambuye Yehova wakamba, ¹⁶ nizafunafuna otayika, na kubwezanso otamangisiwa. Nizamanga zotyoka na kuchilisa zodwala, koma zonenepa na zolimba nizazibononga. nizabeta mwachilungamo. ¹⁷ Manje imwe, nkosa zanga-ichi ndiye chamene Ambuye Yehova akamba-, Onani, nizankhala woweluzi pakati pa nkhusa na nkhusa, na pakati pa nkhusa zamphongo na mbuzi. ¹⁸ Naga sikukwanila kudya musipu wabwino, kuti mudyakilile pansu na mendo yano zossala za musipu; na kumwa manzi oyela, kuti mumatipa mumimana na mendo yano? ¹⁹ Kodi nkhusa zanga ziyenela kudya zimene mwadyakadyaka na mendo yano, na kumwa zamene mwaziponda na mendo yano? ²⁰ Ndiponso Ambuye Yehova akamba izi kuli beve: Onani! Ine neka nizaweluzi pakati pa nkosa zoina na zoyonda, ²¹ popeza munaziponda na nthiti zanu na mapewa yano, ndipo zofoka zonse mwapaya na minyanga zanu, mpaka mwazimwaza kuzichosa muziko. ²² Nizapuluma nkhusa zanga, ndipo sizizankalanso zodyakiliwa, ndipo nizaweluzi pakati pa nkhusa na nkhusa. ²³ Nizaika mubusa umozi, mutumiki wanga Davide. Eve azazibeta, azazidyesa, ndipo azankala mubusa wawo. ²⁴ Pakuti ine Yehova nizankala Mulungu wawo, ndipo mutumiki wanga Davide azankala kalonga pakati pawo, ine Yehova nakamba zamene izi. ²⁵ Pamenepo nizapangana nao chipangano cha mutendele, na kuchosa vilombo voipa muziko, kuti bankhale bochingiliziwa muchipululu, na kugona munkhalango; ²⁶ Nizabwelesa futi madaliso pa beve na mumalo yozungulila phili langa, chifukwa nizagwesa mvula pa nthawi yake. Iyi izankhala mvula yamadalitso. ²⁷ Pamenepo mitengo ya musanga izabala vipaso vake, na ntaka izapeleka vipaso vake. Nkhosa zanga zizankhazikika muziko yawo; pamenepo bazaziba kuti Ine ndine Yehova, pamene nityola mipilingizo ya goli yawo, na pamene nizabapuluma kuchoka mumanja ya bamene babavutisa. ²⁸ Sizizankalanso zodyewa za maziko, na nyama zamusanga paziko lapansi siizabadyanso. Pakuti bazankala mosatekeseka, ndipo palibe wamene azabayofya. ²⁹ Chifukwa nizabapasa ziko yozibika na vipaso vake; ndipo sibazankhala bakufa na njala muziko, ndipo sibazanyozewa na maziko. ³⁰ Ndipo bazaziba kuti Ine, Yehova Mulungu wawo, nili nabeve. Nibantu banga, nyumba ya Isiraeli, uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova. ³¹ Chifukwa imwe ndimwe nkhusa zanga, nkhusa za musipu wanga, na banthu banga, na ine ndine Mulungu wano, uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova.”

Chapter 41

¹ Ndipo mwamuna ananibwelesa mu tempele mumalo yoyela na kupima mafelemu ya pakomo- mikono isanu na umoji kumbali zonse. ² Muufupi mwake mwa pakomo mikono khumi; Koma lakumbali zonse inali mikono isanu muutali mwake. Ndipo munthu uyo anapima mwambili mwa malo yopatulika, mikono 40 muutali, mikono 20 muufupi. ³ Ndipo mwamuna anangena mu mumalo yopatulika kwambili na nakupima nsenamila za zipatazo zinali mikono ibili, na muufupi mwake munali mikono 6. Makomo kumbali zonse zibili anali mikono 7 muufupi. ⁴ Ndipo anapima muutali mwake mikono 20. Muufupi mwake munali mikono 20 kusogolo kwa Nyumba ya Mulungu. Ndipo anati kwa ine, Aya ni Malo yopatulika. ⁵ Mwamuna anapima chipupa cha nyumba- inali 6 mikomo yotikama. Muufupi mwa chipinda chilichonse cha mumbali mwa nyumba, muufupi mwake munali mikono inayi. ⁶ Munali vipinda va mumbali vitatu, chipinda chimozi pamwamba pa chinzake, vipinda makumi yatatu mumalo yaliyonse. Panali visulo vochingilila vipinda vonse va mumbali, popeza panalibe vogwililila chipupa va nyumba. ⁷ Koma vipinda vamumbala vinakula na nazungulila pokwelelapo, chifukwa nyumba inayenda mozungulila pamwamba na pamwamba kuzunguluka monse; vipinda vinakula pamene nyumba inayenda pamwamba, na pokwelela yanayenda pamwambapamalo yenangu, kupitila pamalo ya pakati. ⁸ Ndipo ninaona yokwela malo yozungulila nyumba, na maziko ya mumbali mwa vipinda vamumbali; Iye anapima kamtengo kathunthu m'litali mwake mikono isanu ndi umodzi. ⁹ Muufupi linga la zipinda zamumbali kunja kwake linali mikono isanu. Panali malo yoseguka kunja kwa zipinda zimenezi mumalo yopatulika. ¹⁰ Kumbali inangu ya aya malo panali vipinda vakunja va bansembe; malo yamene ayo yanali mikono makumi awili muufupi mwake pozungulila pa malo yopatulika. ¹¹ Panali viseko va muvipinda va mumbali zotuluka mumalo yena yoseguka. Muufupi mwa bwalo ya mumeneli inali mikono isanu kuzungulila. ¹² Chomanga chamene chinali kulanganana naku bwalo kwa kumazulo inali mikono 70 muufupi mwake. Khoma lake linali lalitali mikono isanu mozungulila, ndipo m'litali mwake linali mikono 90. ¹³ Ndipo mwamuna anapima malo yopatulika, muutali mwake mikono zana limozi. Nyumba yopatuliwa, vipupa vake, na bwalo nayonso inapimidwa mikono zana muutali mwake; ¹⁴ Muufupi mwake mwa kusogolo kwa bwalo mu malo yopatulika munali mikono zana limozi. ¹⁵ Ndiponso mwamuna anapima utali wa nyumba kuseli kwa malo yopatulika chakumazulo kwake, na makonde kumbali iliyonse- 100 mikono. Malo yopatulika na khonde, ¹⁶ Vipupa vamukati na mazenela, na mazenela yang'ono yang'ono, na makonde kuzungulila mbali zitatu, zonse banazikonkomela na mapulanga. ¹⁷ Pamwamba pa khomo yongenelamo muchipinda chamukati mu malo yoyela na chotalamukila kupita muvipupa kuja nichisanzo chakupima. ¹⁸ Inakongolesewa na akerubi na mutengo wa kanjeza; na mutengo wa kanjeza pakati pa kerubi aliyense, na kerubi aliyense anali na nkope zibili: ¹⁹ nkope ya muntu inayangana ku mutengo wa kanjeza kumbali imozi, na nkope ya mukango ung'ono inayangana ku mutengo wakanjeza kumbali yina. Anajambula mozungulila nyumba yonse. ²⁰ Kuchokela pansi mpaka pamwamba pa komo, akerubi na mitengo ya kanjeza anajambula panja pachipupa chakunja kwa nyumba. ²¹ Chipata cha malo oyela chinali lalikulu. Maonekedwe yawo anali ngati mawonekedwe a ²² guwa la maluba pasogolo pa malo oyela, omwe anali mikono itatu mikono itatu na mikono ibili m'litali mbali iliyonse. Pakona wake, maziko, na chimango adapangidwa ndi mitengo. Ndipo mwamunayo anati kwa ine, ili ndiye tebulo loyimilila pamaso pa Yehova. ²³ Kunali viseko vibili za malo oyela na malo oyela kwambili. ²⁴ Zitseko izi zidakhalala na mapanelo abili bomwe anali ndi ziweto zibili zilizonse pakomo limozi na mapanelo abili. ²⁵ Paviseko va malo yopatulika- panali akerubi na mitengo ya kanjeza monga mwamene bana wonesela bwino pa makomo, ndipo pakondepo panali denga lamatabwa. ²⁶ Panali mazenela yopapatiza na mitengo ya kanjeza kumbali zonse za kondelo. Ivi vinali vipinda va mumbali mwa nyumba, ndipo madenga yanali yolenjeka kwambili.

Chapter 43

¹ Ndipo mwamuna ananibwelesa ku chipata chamene chinaseguka chakumumawa. ² Onani! Ulemelelo wa Mulungu wa Israyeli unachokea kumumawa; mau yake yanali ngati chikokomo cha manzi yambili, nda ziko lapansi linawala na ulemelelo wake. ³ Kunali kolingana mu maonekedwe ya masomphenya yamene ninaona, monga masomphenya ninaona pamene anabwela mu kuononga muzinda, ndipo masomphenya yanali monga masomphenya yamene ninaona kumumana wa Kebara canal-ndipo ninagwesa nkope yanga pansi. ⁴ Ndipo ulemelelo wa Yehova unafika ku nyumba kuchokela ku chipata chosegula chakumumawa. ⁵ Pamenepo muzimu unaninyamula na kunibwelesa mukati mwa bwalo lamukati. Onani! Ulemelelo wa Yehova unali kuzulisa nyumba. ⁶ Mwamuna anaimilila pambali panga, ndipo ndinanvela munthu winangu akamba naine kuchokela mnyumba. ⁷ Ananiuza kuti, "Mwana wamunthu, yano ni malo ya pamupando wanga pano ndi malo a mpando wanga wachifumu, na podyakapo mendo yanga, mumene nizankhala pakati pa bana a Israyeli kosatha. Nyumba ya Isiraeli siizaipasa zina langa loyela, beve kapena mafumu yawo na kusakhulupilika kwawo, kapena na mitembo ya mafumu yawo pamisanje yawo. ⁸ Sibazaipisa zina langa loyela, na kuika pakhomo yao pafupi na pakhomo yanga, na mphuthu zao pafupi ndi mphuthu za zipata zanga, popanda kalikonse koma pakati pa ine na beve. Banaipisa zina langa loyela na zonyansa zao, ndipo ninawatha na ukali wanga. ⁹ Manje lekani bachosepo kusakulupilila kwawo na vitumbi va mafumu yawo pamenso panga, ndipo nizankhala pakati pawo muyayaya. ¹⁰ Mwana wa munthu, iwe weka ufunika uuze nyumba ya Israyeli za nyumba iyi kuti bankale na manyazi na zolakwa zao. Bafunika kuganizila pali uku za kufotokoza. ¹¹ Chifukwa bakankala na manyazi pali vonse vamene bachita, pamenepo bavubulusile mamangidwe ya nyumba, zofunikila zake, mochokela panja mwake, mongenela mukati mwake, mamangidwe yake yonse, malemba yake yonse na malamulo yake. Ulembe zamene izi pamenso pao, kuti basunge mamangidwe yake yonse, na malemba yake yonse, kuti bayasunge. ¹² Aya ndiye malamulo yamu nyumba: Kuyambila pamwamba pa phili mpaka malile yonse yozungulila nyumba, izankala yoyela. Onani! Aya ndiyo malamulo yapanyumba. ¹³ Aya ndiye makomo ya guwa mu mukomo, mukono umozi, na mukono umozi, muutali mwake na mukono umozi. Kuti ngalande yozungulila guwalo inkhale yakuya mukono umozi, na muufupi mwake mkono umozi. Malire ozungulira m'mpheapete mwake akhale chikhatho chimozi. Pazakhala tsinde la guwa la nsembelo. ¹⁴ Kuchokera mungalande mpaka pansi pa guwa lansembe pali mikono iwili, ndipo mumbali mwake munali mukono umozi. Ndiyenso kuchokela pamphambano waungono kukafika mumbali waukulu wa guwa lansembe, inali mikono inayi, ndipo mumbali mwake munali mukono umozi. ¹⁵ Ulemu wa pa guwa lansembe zopseleza utalika mikono inayi, ndipo pali minyanga zinayi zolozza mumwamba pa nganjo. ¹⁶ Muutali mwake mikono 12 na mikono 12 muufupi, mbali zonse zinayi. ¹⁷ Malile yake ndiwo mikono khumi na inai muutali, na mikono khumi na inai mufupi mbali zake zonse zinayi, na mukombelo wake na theka la mukono muufupi. Ngalande inkhale mukono umozi muufupi mwake, ndipo makwelelo yake yanayangana kumumawa. ¹⁸ Pamenepo ananiuza kuti, mwana wa munthu, Ambuye Yehova : "Malamulo a guwa la nsembe pa tsiku la kulipanga ndi awa, a kukwezelapo nsembe yopsereza, ndi kuwazapo mwazi; ¹⁹ Uzipeleka ng'ombe yaing'ono yamphongo monga nsembe yamachimo kwa ansembe Achilevi, ana a Zadoki, yamene akuyandikira kwa ine kunditumikira-uku ndiye kukamba kwa Ambuye Yehova. ²⁰ Pamenepo utengeko mwazi wake, na kuupaka pa minyanga zinai za guwa la nsembe, na mumbali yake zinayi za mumbali mwake, na mumbali mwake; uliyelese na kuchita chotetezela. ²¹ Kenako utenge ng'ombe yamphongo ya nsembe yauchimo na kuitentha pamalo oikidwilatu a Kachisi kunja kwa malo opatulika. ²² Ndipo siku lachiwili uzipoleka mbuzi yamphongo yopanda chilema, inkhale nsembe yauchimo; bansembe baziyeselele guwa monga mwamene anayelesela na ng'ombe yamphongo. ²³ Mukamaliza kuliyelele, muzipeleka ng'ombe yamphongo yopanda chilema, na nkhusa yamphongo yopanda chilema ya mugulu ya nkhusa. ²⁴ Uzipeleke pamenso pa Yehova; bansembe bazithila muchele pa izo, na kuzipeleka nsembe kwa Yehova. ²⁵ Mufunika kukonza mbuzi imuna monga nsembe yamachimo siku iliyonse kwa masiku 7, ndipo bansembe bazipelekanso ng'ombe yamphongo yopanda chilema na nkhusa yamphongo yopanda chilema. ²⁶ Aziphimba machimo a guwalo masiku 7 ndi kuliyeretsa. ²⁷ Ayenela kusiliza masiku aya, na pa siku lachisanu ndi chitatu na musogolo, bansembe bazakonzelatu nsembe zanu zopseleza na nsembe zanu zamtendere paguwa lansembe; ndipo nizavomeleza imwe, akamba Ambuye Yehova.

Chapter 47

¹ Pamene apo mwamuna uyo ananibweza futi pongenela pa nyumba ya mulungu; ndipo penze manzi yenze kuchoka pansi pa chiwunda cha nyumba ya mulungu, chakumawa, chakusogolo kwa nyumba ya mulungu, na manzi yenzoyenda kumwela kwa nyumba ya mulungu, kukwanja yamanja ya guwa ya nsembe. ² Chifukwa cha icho ananichosela popitila chakumpoto, nakunizungulila mpaka kopitila koyangana kumawa. ³ Pamene muntu uyo enze kumawa, enze na ntambo yo pimila mumanjikuyenda a mwake; Anapima mikono 1,000, ananipoisha mumanzi umo mpaka manzi kuyamba kuyenda mumendo. ⁴ Pamene apo anapima futi mikono cikwi cimozi, nakunipisha mumanzi umo mpaka manzi kuyamba kuyenda mumendo; futi anapima futi mikono 1,000 nakuyenda naine kumanzi yoyenda mumusana. ⁵ futi anapima futi mikono 1,000, koma wenze mumana wamene sininga kwanise ku tawuka, chifukwa manzi yenze yana kwela, ndipo wenze wozama wakuti muntu angasambilemomo, ndipo wenze musinje wosakwanisika kutauka. ⁶ Muntu uyo ananifunsa ati: “Iwe mwana wa muntu, mwati uviwona ivi?” ⁷ futi ananichosa nakunipitisa mumbali mbali mwa mumana wamene uyu. ⁸ Muntu uyo anakamba kuli ine, manzi aya yachoka kuyenda kumalile ya kumawa, nakuselukila ku Araba; manzi aya ayenda munyanja ya sawuti, nakuyi panga ya bwino. ⁹ Ndiye pamene kuzapezeka kuti vamoyo vonse vokalaba vizankala na kwamene; pazankala nsomba zambili, chifukwa manzi aya yayenda mwamene umo. zizapangisa manzi ya sawuti kunkala yabwino. Chilichonse chizankala na moyo kulikonse kwamene mumana wamene uyu uyenda. ¹⁰ Pamene apo kuzapezeka kuti bogwila nsomba baku Eni-Gedi bazayimilila mumbali mbali mwa manzi yamene ayo, ndipo pazankala poyanikila vogwilila nsomba ku Eni-Egilaimu. Pazankala nsomba zambili za munyanja za sawuti monga nsomba za munyanja yikulu chifukwa chokupaka kwa kayena. ¹¹ Koma madambo na madambo ya Nyanja ya sawuti sivizachinjiwa; yazankala yopasa sawuti. ¹² Pambali pa mumana uyu mumbali mbali mwakayena, mbali zonse zibili, pazankala mitengo yosiyanasiyana yobala vakudya. Matepo yawo siyaza fota, ndipo vipaso vake sivizakakangiwa kukula. Mwezi uliwonse mitengo iyo izabala vipaso chifukwa manzi yochoka mumalo yopatulika yamapitako. vipaso vake vizakankala vakudya, ndipo matepo yake yazankala yopolesa. ¹³ Akamba Ambuye Yehova, ndiye mwamene uzagabanisila ziko mitudu kumi na yibili ya Israyeli: Yosefe azankala na magawo yabili. ¹⁴ Mugabane molingana na vamene ninakwezekea kwanja yanga na kulapa kuti nizapasa makolo yanu. ziko iyi izabwela kuli imwe monga choloba chanu. ¹⁵ Yamene aya ndiye malile ya kumupoto, kuchoka ku Nyanja Yikulu kuyenda ku Heteloni, na ku Zedadi. ¹⁶ Ndipo malile yamene ayo yazafika ku Berota, mpaka ku Sibraimu, yamene ili pakati pa Damasiko na Hamati, mpaka ku Hazeri Hatikoni yamene ili mumbalimbali mwa malile ya Haurani. ¹⁷ Chifukwa cha icho malile yamene ayo yayambile ku nyanja kuyendo fika ku Hazara Enani, na Damasiko na ku Hamati, kumupoto. Iyi ni mbali ya kumupoto. ¹⁸ Kumawa, malile ayo ayambile pakati pa Haurani na Damasiko, na mumana wa Yolodani, pakati pa Giliyadi na ziko ya Isiraeli. Mupime kuyambila kumalile kuyenda kufika ku nyanja ya kumumawa. yamene aya ndiye yankale malile ya kumumawa. ¹⁹ Kumbali ya kumwela, malile yamene ayo ayambile ku Tamara kuyenda kufika kumanzi ya Meriba Kadesi, na kumusinje wa Aiguputo mpaka ku Nyanja Yikulu. yamene aya ndiye yankale malile ya kumwela. ²⁰ futi malile ya kumazulo yankale Nyanja yikulu kuyendo fika kuyenda kufika kusogolo kwa Lebo Hamati. Iyi izankala mbali ya kumazulu. ²¹ Mwamene muzagabila ziko ili ku ba mitundu ya Israele. ²² mwa ichi mugabane cholowa chanu na balendo bamene bali pakati panu, bamene babala bana pakati panu, bamene bali pamozi na imwe, monga mwamene bana badwila ku Isiraeli. Muzachita mayele pakati pa mitundu ya Isiraeli. ²³ Pamene apo mulendo azankala pamozi na mutundu wamene unkala nawo. Umupase choloba chake, Akamba YEHOVA, Ambuye Mukulu .

Daniel

Chapter 6

¹ Chinaooneka chabwino kuli Dariusi kusankha bolamulila zigawo 120 kuti azilamulila ufumu uyo. ² Pali beve panali bakulu boyanganila nchito batatu, ndipo Danieli anali umodzi wa beve. Bakulu boyanganila bamene banasankiwa kuti aziyangana bolamulila azigawo, kuti mfumu isatayike. ³ Danieli anali wolemekezeka kuchila bakulu boyanganila nchito bena bonse na bolamulila azigawo chifukwa anali na muzimu wodabwisa. Ba mfumu banali kulinganiza kumuika kunkhala woyanganila ufumu wonse. ⁴ Pameneapo bena bakulu boyanganila nchito na bolamulila azigawo anayangana zolakwila pa nchito yamene Danieli anagwila pa ufumu, koma sibanapeze

kubosha kapena kulepela pa nchito yake chifukwa anali wokhulupilika. Palibe zolakwa kapena kosasamala kunapezeka muli eve. ⁵ Pameneapo bamuna aba banakamba kuti, "Sitingapeze chifukwa chili chonse cha kudandaulila Danieli wamene uyu, ngati sitipeza kanthu koshushana naye pa chilamulo cha Mulungu wake." ⁶ Pameneapo bakulu boyanganila nchito na bolamulila banabwelesa ganizo pamanso pa mfumu. Ndipo banati kuli eve, 'Mfumu Dariusi, munkhale na umoyo osatha! ⁷ Bonse bakulu boyanganila nchito yamu ufumu, bolamulila malo azigawo, na bolamulila madela, opasazelu, bolamulila bapangana pamodzi, ndipo banagamula kuti imwe, mfumu, mupeleke lamulo naku kazikisa lamulo yolesa, kuti aliyense wopempa kuti apeleke lamulo, mulungu ali yense kapena munthu masiku makumi yatatu, koma kwa imwe, mfumu, munthu uyu adzaponyewa muzenje ya mikango. ⁸ Manje, mfumu, pelekani lamulo naku saina chikalata kuti sichizachingiwa, monga kuongolela malamulo ya Medes na Persians, kuti sichichosewa. ⁹ Mfumu Dariusi anasaina chikalata, kuti chinkhale lamulo. ¹⁰ Pamene Danieli anazeba kuti chikalata chasainiwa kuti chinkhale lamulo, anagena munyumba yake (manje mazenela yake anali osegula muchipinda chake chapamwamba kuyangana ku Yerusalemu), ndipo anagwada pansi, monga mwamene amachitila katatu pasiku, anapempela naku yamika pamanso pa Mulungu wake, monga anachita kale. ¹¹ Pameneapo bamuna bamene banakonza chiwembu pamodzi banaona Danieli apempa nakufuna thandizo kuchokela kwa Mulungu. ¹² Ndipo beve banafika kwa mfumu nakukamba na eve za lamulo yake: Kodi simuna pange lamulo kuti aliyense akapemphela kuli mulungu kapena munthu masiku makumi yatatu, koma kwa imwe, mfumu, akaponyewe muzenje yamu mikango?" Mfumu anayankha, "Nkhani iyi yakazikika, monga mwa lamulo ya Amedi na Aperisi; sichingachosewe. ¹³ Pameneapo banati kuli mfumu, "Munthu uyo Danieli, ndiye umodzi wa banthu ocokela ku Yuda, sakumvelelani imwe, mfumu, kapena lamulo yamene munalemba. Eve amapempela kuli Mulungu wake katatu pasiku." ¹⁴ Mfumu pamene anamvela zamene izi, anakalipa kwambili, ndipo anayesa kupulumusa Danieli ku lamulo yamene iyi. Eve anayesayesa mpaka kulowa kwa zuba kuti apulumuse Danieli. ¹⁵ Pameneapo bamuna bamene banapanga chiwembu banasonkhana pamodzi na mfumu nakukamba kuti kuli eve, "Zibani, mfumu, kuti iyi ni lamulo ya Amedi na Aperisi, kuti lamulo iliyonse kapena lamulo iliyonse yamene mfumu afaka sigachinjiwe. ¹⁶ Pameneapo mfumu analamula, ndipo anabwelesa Danieli, naku munponya muzenje ya mikango. Mfumu anakamba kuli Danieli, 'Mulungu wako, wamene umtumikila kosalekeza, akupulumuse. ¹⁷ Mwala unafika pakomo ya dzenjelo, ndipo mfumu inadindapo na mphete ya keyake na mphete za olemkezeke zake kuti kulibe chilichonse chochita kuli Danieli. ¹⁸ Pameneapo mfumu anayenda kunyumba yake yachifumu. Ndipo usiku wonse sanadye chokudya chilichonse. Palibe chosangalasa chamene chinabwelesewa pamanso pake, ndipo tulo tunamutaba. ¹⁹ Mukucha kwakuseni, ba mfumu bananyamuka nakupita mofulumila kuzenje ya mikango. ²⁰ Pamene anabwela pafupi zenjelo, anayitana Danieli na mawu yachisoni, anati kuli Danieli, "Danieli, wanchito wa Mulungu wamoyo, kodi Mulungu wako, wamene umtumikila kosalekeza, akwanisa kukupulumusa ku mikango?" ²¹ Pameneapo Danieli anakamba kuli mfumu, "Mfumu, nkhalani na umoyo wamuyayaya!" ²² Mulungu wanga atumiza mutumiki wake nakuvala pakamwa pa mikango, ndipo sivilinichite ine. Pakuti ninapezeka wopanda cholakwa pamanso pake na pamanso panu, mfumu, ndipo ine sininakuchitileni choipa chilichonse. ²³ Kenako mfumu inasangalala kwambili. Eve analamula kuti bamuchose Danieli muzenjemo. Chotero Danieli banamuchosa muzenjemo. Palibe choipa chamene chinapezeka pali eve, chifukwa anakulupilila Mulungu wake. ²⁴ Mfumu inalamula, ndipo banabwelesa bamuna bamene bananenela Danieli na kubaponya muzenje ya mikango - beve, bana bawo, na makazi bawo. Bakalibe kufika pansi, mikango inabagonjeza ndipo inathyola mafupa yawo bonse kunkhala zidunswazidunswa. ²⁵ Pameneapo mfumu Dariusi analembela banthu ba mitundu yonse, mitundu, na manenedwe yonkhala paziko yonse yapansi: "Mtendere ukuchulukile imwe. ²⁶ Cifukwa cake naika lamulo kuti mumaike yonse a ufumu yanga banthu anjenjemele na kuyopa pamanso pa Mulungu wa Danieli, pakuti eve ndiye Mulungu wamoyo wakunkhala na umoyo wamuyayaya, na ufumu wake suzaonongeka; ulamulilo wake uzankhala kufikila chimalizilo. ²⁷ Eve amatiteteza nakutipulumusa, ndipo amachita zizindikilo na zoziba kumwamba na paziko yapansi; wateteza Danieli ku mphamvu ya mikango." ²⁸ Choncho vinthu vinamuyendela bwino Danieli mu ulamulilo wa Dariusi namu ulamulilo wa Koresi Mperisi.

Chapter 7

¹ Muchaka choyamba cha ulamulilo wa Belisazara mfumu yaku Babulo, Danieli analota maloto na mensompenya pamene anagona pabedi yake. ndipo analemba analemba vamene anawona mumaloto. eve analemba vintu vofunika kwambili vamene vizachitika:

² Danieli anakamba ati: “Mumasompenya yanga usiku ninawona mphepo ³ zinayi zakumwamba ninshi zivundula nyanja. ⁴ Yoyamba yenze monga nkalamu koma yenze na mapapiko ya chiwombankanga. Pamene nenze kuyangana, mapapiko yake yana tyolewa ndipo inanyamuliwa pansi na kuyi imika na mendo yabili monga muntu. Maganizo ya muntu yanapasiwa kuli beve. ⁵ Ndiponso penze nyama yachibili, ili monga chimbalingondo, yamene yenze kubelama. mukamwa mwake mwenze mbambo zitatu pakati pa meno yake. Ana uziwa kuti, 'Nyamuka udye banthu bambili.' ⁶ Pamene vinasila ivi nina yangana futi. Penze futi nyama inango yo woneka monga kayingo. Kumusana kwake chenze na mapapiko yanayi yali monga mapapiko ya nyoni, ndipo chenze na mitu mitu inayi. Anapasiwa ulamulio wolamulia. ⁷ pamene vinasila ivi ninawona mumesompenya ya usiku chilombo cha chinayi, choyofya, futi cha mpamvu maningi. chenze nayo meno yakulu yachisulo; inapwanya, kudya, nakudyakadyaka vinasalako. chenze chosiyana na nyama zinango, chenze na nsengo kumi. ⁸ Pamene nenze kuganizila pa nyanga zamene izo, ndipo ninaona nyanga inango imela pakati pa zeve, nyanga ing'ono. Nyanga zitatu pali nyanga zija zina nyuliwa na mizyu. Ninaona menso mu nyanga yamene iyi monga menso ya muntu na pakamwa pozimvela vintu vikulu vikulu. ⁹ Pamene ninaona, mipando ya ufumu yamene yinankazikisiwa, ndipo nkalamba inankala pa mupando wake. vovala vake venze voyela monga matalala, ndipo sisi ya pamutu pake yenze yenze monga usako wa nkosa yoyela. Mupando wake wa ufumu wenze malasha ya mulilo, ndipo mawilo yake yenze mulilo woyaka. ¹⁰ Mumana wa mulilo una choka pamenso pake ; bantu mamiliyoni yambili yenze kumutumikila, ndipo bantu 100 miliyoni bana imilila pamenso pake. ndipo Koti yenze mukati, ndipo mabuku yanaseguliwa. ¹¹ Ninapitiliza kuyang'ana chifukwa cha mawu yozitukumula yana kambiwa na nyanga iyo. Ninaona pamene chilombo icho chenze kupaiwa, ndipo mutembo wake unawonongewa, ndipo unayendo shokewa. ¹² Ndipo pali nyama zinango zinayi zija, ulamulio wao wo lamulila unachosewa, koma moyo wawo unatalimpisiwa kwa ka ntaŵi. ¹³ Mumenso mphenya yanga usiku wamene uyo, ninaona winango abwela na makumbi ya kumwamba monga mwana wa muntu; anabwela ku nkalamba ya kudala yamene, na kuonekela pamenso pake. ¹⁴ kulamulila na ulemelelo na mpamvu za ufumu vinapasiwa kuli eve kuti bantu bonse, mitundu yonse, na makambidwe yonse yamutumikile. Ulamulilo wake wo lamulila ni ulamulilo wosasila wamene suzakasilapo, ndipo ufumu wake ni wakuti siwuzakawonongekapo. ¹⁵ Koma ine, Danieli, muzimu wanga unavutika mumutima mwanga, ndipo mensompenya yamene ninaona mumaganizo yanga yananihutisa. ¹⁶ Ninayenda kuli umozi wa beve benze bana imilila na kumupempa kuti anilangize tantauzo ya vintu vamene ivi. ¹⁷ vinyama vikuluvikulu vamene ivi, venze vinayi, nima ufumu ya nayi yamene yaza nyamuka pa ziko yapansi. ¹⁸ Koma bopatulika ba Wamumwambamwamba baza landila ufumu uyo, ndipo azankala nawo mpaka muyayaya. ¹⁹ Pamene apo ninafuna kuziba vambili pa nyama ya chinayi, yosiyana na zinzake na meno yacisulo na njala zake za mukuwa; ina ng'amba ng'mba, kupwanya pwaya, na kudyakadyaka vamene vinasala na mendo yake. ²⁰ Ninafuna kuziba va nyanga kumi pamutu pake, na va nyanga inango yamene inamela, na nyanga zitatu izo zinagwa pasogolo pake. Ninafuna kuziba va nyanga iyo inali ndi maso, ndi pakamwa pa imene inkadzitamandira zinthu zazikulu, imene inkaoneka yaikulu kuposa anzake. ²¹ Pamene ninayangana, nyanga iyi yamene inamenyana na bantu boyela mitima ndipo yenze kubagonjesa ²² mpaka inafika nkalamba yakale, ndipo chilungamo china pasiwa kuli bantu boyela ba Wakumwambamwamba. Dipo inafika ntawi yamene bantu boyela banalandila ufumu uja. ²³ Muntu uja anakamba ati, 'Nyama yachinayi, izankala ufumu wachinayi paziko lapansi wosiyana na maufumu yenango yonse. izadya ziko yonse yapansi, ndipo izai dyakadyaka na kuyipwanyapwaya. ²⁴ Koma za nyanga kumi izo, mu ufumu uyu muza uka mafumu kumi, na pambuyo pabo uza uka winango. eve azankala wosiyana na bakudala, ndipo azagonjesa ma ufumu yatatu ayo. ²⁵ Eve azakamba mau nonyoza wamumwambamwamba ndipo azadyakilila boyela mitima ba mulungu wamumwambamwamba. Azayesa kuchinja vikondwelelo na lamulo. vintu vamene vizapelekewa mumanja muchaka chimozi, zaka zibili, na chaka cha teka. ²⁶ Koma bwalo yamilandu izakhalapo, ndipo beve bazachosa mpamvu zake za ufumu kuti zisilizwe na kuwonongewa pakusiliza kwakayena. ²⁷ Ufumu na ulamulilo, na ukulu wa ma ufumu ya pansi pa mutambo wonse, zizaperekewa ku bantu bopatulika ba Wamumwamba mwamba. Ufumu wake ni ufumu wosasila, ndipo ma ufumu yenango yonse yazamutumikila na kumumvela.' ²⁸ Uku indiye kusila kwankani. Koma ine Danieli, maganizo yanga yananihutisa maningi, ndipo mfeshi yanga inachinja maonekedwe. Koma ninasunga vintu ivi paneka.

Chapter 9

¹ Dariyo anali mwana wa Ahaswero, mbadwa ya Amedi. Anali Ahasiwero bamene anaikidwa kunkala mfumu ya Ababulo. ² Muchaka choyamba cha ufumu wa Dariyo, ine Danieli ninali kuphunzila mumabuku yamene munali mau ya Yehova, yamene yanali kuli mneneli Yeremiya. Ninaona kuti pasala zaka 70 kuti Yerusalemu aonongewe. ³ Nina pindamula nkope yanga kuli Ambuye Yehova, kumfunafuna na pempelo na mapembezo, na ku kudya, kuvala, na kunkala pa masaka na kunkala mu milota. ⁴ Ninapempela kuli Yehova Mulungu wanga, ndipo ninaulula machimo yatu. Nina na kamba, “Niku pempani, Yehova, ndimwe Mulungu mkulu na woopsa, ndimwe bamene mumasunga chipangano na okulupilika kukonda bamene bamakukondani na kusunga malamulo yanu. ⁵ Tachimwa ndipo tachita zoipa. Tachita zoipa, tapanduka, na kupatuka ku malamulo yanu na malemba yanu. ⁶ Sitinamvele batumiki banu baneneli bamene bana kamba muzina yanu kuli mafumu yatu, asogoleli batu, makolo batu, na kuli bantu bonse ba mziko. ⁷ Kuli imwe, Yehova chilungamo ni chanu, kuli ise lelo tili na manyazi pankope zathu, kuli bana ba Yuda, onkala mu Yerusalemu, na Isiraeli onse. Kufakapo nabaja bali pafupi na bamene bali kutali mumaziko yonse kwamene munabmwazikanya. Nichifukwa cha chinyengo chachikulu chamene takuchitilani. ⁸ Ise, Yehova, tili na manyazi pankope zathu, kuli mafumu yatu, na asogoleli yatu, na makolo yatu, popeza takuchimwilani. ⁹ Kuli Yehova Mulungu watu kuli chifundo na chikhululukilo, pakuti tampandukila. ¹⁰ Sitinamvele mau ya Yehova Mulungu watu mukuyenda mumalamulo yake yamene anatipasa kupitila muli batumiki bake baneneli. ¹¹ Baisraeli bonse balakwila chilamulo chanu, napatuka, osamvela mau yanu. Tembelelo na lumbilo yolembewa muchilamulo cha Mose, mtumiki wa Mulungu, batalia pali ise, chifukwa tamchimwila. ¹² Yehova asimikiza mau yamene ananena moshushana na ise na olamulila yatu, ni kutibwelesla soka ikulu. Chifukwa pansi pa tambo yonse yapansi sipanachitikepo chilichonse kulinganiza na vamene vinachitikila Yerusalemu. ¹³ Monga mwamene zinalembewela muchilamulo cha Mose, soka yonse yatigwela, koma sitinapempele Yehova Mulungu watu kuti atichitile chifundo mukuleka mpulupulu zathu na kuikila nzelu ku ch chazona chatu. ¹⁴ Mwaicho Yehova wakonzelatu sokalo ndipo atibwelesela, chifukwa Yehova Mulungu watu na bolungama muzochita zake zonse, koma ise sitinamvele mau yake. ¹⁵ Manje, Yehova Mulungu watu, munachosa bantu banu muziko ya Igupto na kwanja yampamvu, ndipo munazipangila mbili, monga siko yalelo. Koma ise tinachimwa; tachita zoipa. ¹⁶ Yehova, chifukwa cha ntchito zanu zonse zolungama, kukalipa kwanu na ukali wanu zichoke pa mzinda wanu Yerusalemu, lupili yanu yopatulika. Chifukwa cha machimo yatu, chifukwa cha mpulupulu za makolo yatu, Yerusalemu na bantu banu bankala chintu chonyozeka na bonse otizungulila. ¹⁷ Manje, Mulungu watu, nvelani pempelo ya kapolo wanu, na kupempa kwake mozichipea; chifukwa cha imwe, Yehova, muwalise nkope yanu pa malo yanu yopatulika yamene yali bwinja. ¹⁸ Mulungu wanga, segulani matu yanu, munvele; segulani menso yanu muone. Tatedwa nzelu; yanganani munzi wamene uitaniwa na zina yanu. Sitipempa kuzichepesa kwatu kuli imwe chifukwa cha chilungamo chatu, koma chifukwa cha chifundo chanu chachikulu. ¹⁹ Ambuye, nvelani! Ambuye, kululukilani! Ambuye, ikankoni nzelu na kuchitapo chintu! Chifukwa cha imwe, musachedwe, Mulungu wanga, chifukwai munzi wanu na bantu banu baitaniwa na zina yanu. ²⁰ Pamene ninali kukamba- kupempela na ku ulula chimo changa, na chimo cha bantu banga Israeli, na kupeleka zopempa zanga pamenso pa Yehova Mulungu wanga, pa lupili yopatulika ya Mulungu; ²¹ pamene ninali kupempela, muntu Gabrieli, wamene ninamuona mumansompenya poyamba, anaulukila kuli ine motamanga, pa ntawi ya nsembe yamazulo. ²² Ananipasa kuziba na kukamba kuli ine, Daniele, nabwela manje kukupasa chizibiso na kuzibisa. ²³ Pamene munayamba kulangiza kupempa kwachifundo chanu, lamulo inapasiwa, ndipo nabwela kukuuzani yanko, chifukwa mumakondewa kwambili. Mwaicho lingalilani mau aya, na kunvesesa chivumbuluso. ²⁴ Makumi yasanu na yabili mpambu yisanu na yibili yalamuliwa ku bantu bako na mzinda wako bopatulika kuti asayese mpulupulu na kutesa chimo, kutetezela choipa, kubwelesela chilungamo chamuyaya, kuchita mansompenya na ulosi, na kuyeleza malo yopatulika kwambili. ²⁵ Zibani na kumvesa kuti kuyambila pa kupelekewa ku lamulo yokonza na kumanga Yerusalemu mpaka kubwela kwa wozozewa (wamene azankala musogoleli), pazankala zisanu na zibili, makumi yasanu na imozi mphambu zibili. Yerusalemu izamangiwa nafuti na njila na ngalande, mosasamala kantu ya ntawi ya masauso. ²⁶ Pambuyo pa zaka 62, wodzozedwayo adzawonongedwa ndipo sadzakhala ndi kalikonse. Gulu lankhondo la wolamulira amene akubwera lidzawononga mzinda ndi malo opatulikawo. Mapeto ake adzadza ndi chigumula, ndipo padzakhala nkondo mpaka mapeto. Zipululu zalamulidwa. ²⁷ Azakavomeleza chipangano naba mbili pali 7. Pakati pabali 7 aza siliza chopeleka na cha nsembe. Pa papiko ya zonyansa pazabwela wina bamene ba nonga mpaka chionongeko chosiliza chamene chakambiwa chatiliwa pali wamene abwelesela ku ononga.’

Joel

Chapter 1

¹ Aya ndiye mau ya Mulungu yamene yanabwela kuli Yoweli mwana mwamuna wa Petueli. ² Nvelani ichi, imwe bazikulu, naku nvesesa, imwe bonse bonkala mumalo. Nanga kuna chitikapo chaso muma siku yanu kapena muma siku yama kolo banu? ³ Uzani banu pali ichi, ndipo lekani bana banu bauze bana bao, na bana bao bauze mibadwo zobwelapo. ⁴ Vamene gulu ya ntete yasiya, ntete zikulu zadya; vamene ntete zikulu zasiya, sontwa zadya; ndipo vamene sontwa zasiya, vinkubala vadya. ⁵ Ukani, imwe okolewa, naku lila! pundani, imwe bonse bokumwa vinyu, chifukwa vinyu yonveka bwino yachosewa kuchokela kuli imwe. ⁶ pakuti mutundu wabwela muziko yanga, olimba naulibe chibelengelo. Meno yake nimenyo ya nkalamu, ndipo alina meno monga yankalamu ikazi. ⁷ Alengesa mpesa yanga kunkala malo yoonongeka naku ukushuba mukuyu wanga. Ashuba chikamba chake naku chitaya; ntambi zake zasanduka zotuba. ⁸ Lilani ngati namwali ali vale vovala vama saka pakufa kwa bamuna bake bachi nyamata. ⁹ Chopeleka chaunga nachopeleka chakumwa vachosewa ku chokela mu nyumba ya Yehova. Wansembe, kapolo wa Yehova, alila. ¹⁰ Minda zaonongewa; pansi pa lila chifukwa mbeu zaonongewa. vinyu yasopano ya yayuma; mafuta yataika. ¹¹ Nkalani bansoni, imwe balimi, lilani mopunda, imwe olima mpesa, chifukwa cha tiligu na barlele. Pakuti vokolola vamu munda vaonongeka. ¹² Mpesa za fota ndipo mitengo zamukuyu zayuma; mitengo za mukangaza, namitengo zakanjeza, na mitengo zama apulo_ mitengo zamu munda zonse za fota. Pakuti chimwemwe cha chosewapo kuchokela mumi badwo wa muntu. ¹³ Valani vovala vama saka na kulila modandaula, imwe bansembe! lilani, imwe banchito bapa guwa. Bwelani, gonani muvovala vamasaka usiku onse, imwe banchito ba Mulungu wanga. Chifukwa chopeleka cha chimanga nachopela cha chakumwa valesewa mu nyumba ya Mulungu. ¹⁴ Itanisani siku yaku sala kudya koyela, nakuitanisa kusonkana koyela. Sonkanizani bazikulu nabonse bonkala mumalo ya munyumba ya Yehova Mulungu wanu, nakulilila kuli Yehova. ¹⁵ Iyee siku iyi! Pakuti siku ya Yehova ilipa fupi na kufika. Izabwela nachionongeko kuchokela kuli Wampanvu zonse. ¹⁶ Nanga sichina chosewe chakudya kuchokela pamenso yatu, na chisangalalo na kukondwela kuchokela mu nyumba ya Mulungu watu? ¹⁷ Mbewu zina ola mukati mwa vikamba vake, mosungila mbewu mwapasuka, na nkokwe zaka zaonongewa, pakuti chimanga cha fota. ¹⁸ Monga ngomba zizumila! Magulu yangombe ya enda enda mosokonezeka chifukwa yalibe vakudya. Nayo magulu ya nkosa ya vutika. ¹⁹ Yehova, nilila kuli imwe. Pakuti mulilo wa ononga vakudya vamu chipululu, ndipo kuyaka kwamulilo kwa shoka mitengo zonse zaku tengo. ²⁰ Ngakale nyama za kutengo zililila Imwe, chifukwa misinje ya yuma, ndipo mulilo wa ononga vakudya vamu chipululu.

Chapter 2

¹ Lizani lipenga mu Ziyoni, na chonvekesa choukisa pa pili yanga yoyela! Lekani bonse bonkala muma malo ba gwiliwe na manta, pakuti siku ya Yehova ibewla; zoon, ilipa fupi. ² Nisiku ya nfinzi na mudima, siku ya makumbi na mudima otikama. Monga kucha kwamene ku vinikila pama pili, mutundu ukulu wa mpavu uyandikila. Sikunankalepo mutundu monga uyu, ndipo siuzakankalapo nafuti, ngakale pata pita mu badwo wanga. ³ Mulilo ukudya chili chonse chamene chili pasogolo pake, kumbuyo kwake mulilo oyaka ushoka. Malo yali monga ni munda wa Edeni kusogolo kwake, koma kumbuyo kwake kuli chipululu choonongeka. Zoon, kulibe chiza pulumukamo. ⁴ Maonekedwe ya gulu yali monga niyaba makavalo, ndipo batamanga monga bakavalo bankondo. ⁵ Ba jumpa nachongo monga chaba magaleta pamwamba pama pili, monga chongo chamulilo woyaka woyofya wamene uoononga chiputu, monga gulu yokonzekela kumenya nkondo. ⁶ Paku nkalapo kwao bantu bankala muchisauko napa menso pao pankala po foka. ⁷ Batamanga monga bankondo ba mpavu; bakwela vipupa monga basilikali; bayenda, moyendela pamozi, mosa pwanja mizela. ⁸ Kulibe ngakale umozi wamene amalasa muzake namukondo; bama enda, aliyense mu munjila yake; bama kwanisa kupita mumalo muli zida mosachoka mu malo mwabo. ⁹ Ba tamangila pa mizinda, batamangila pa vipupa, bakwela muma nyumba, naku kupita muma zenela monga baka walala. ¹⁰ Ziko lapansi inyanganya pamanso pao, kumwamba kunjenjema, zuba na mwezi vankazikiwa mu mudima, na nyenyezi zaleka kuwala. ¹¹ Yehova anvekesa liu yake pamanso pa kamu, chifukwa bankondo bake nibambili maningi; pakuti nibolimba, abo bamene ba chita malamulo yake. Pakuti siku ya Yehova nilikulu ndipo niyoyofya maningi. Nindani wamene anga pulumuke? ¹² "koma ngakale manje," Yehova akamba kuti, "Bwelelani kuli ine namitima yanu yonse, salani kudya, lilani, naku dandaula." ¹³ Nangambani mitima yanu osati chabe vovala vanu, ndipo mubwelele kuli Yehova Mulungu wanu. Pakuti nio koma mutima ndipo niwa chifundo, sakumudwa musanga ali nachikondi chonkazikika, ndipo sakonda kuti langa. ¹⁴ Oziba nindani? Nanga anga chinje naku nvela chifundo, nakusiya daliso pali iye, chopeleka cha mbewu na chopeleka chakumwa cha Yehova Mulungu wako? ¹⁵ Lizani lipenga mu Ziyoni, itanisani kusala kudya koyela, 15 naku itanisa kusunzana koyela. ¹⁶ Sonkanisani bantu; itanisani kusunzana koyela. Bankazikiseni pamozi bakulu; sonkanisani bana na bana bamene banyonka. Lekani bamukwatibwi bachoke muvipinda vao, naba mukwati bachoke muvipinda vao. ¹⁷ Lekani bansembe, banchito ba Yehova, balile pakati pa guwa napo ngenela. Lekani bakambe kuti, Yehova, "lekelelani bantu banu, ndipo musaleke cholowa chanu kunkala ngati chosekewa, kuti maziko yazi banyoze. Bazakambila chani pama ziko, 'Mulungu wao alikuti?'" ¹⁸ Pamene apo Yehova anachitila nsanje ziko yake nakubachitila chifundo bantu bake. ¹⁹ Yehova anabayanka bantu bake kuti, "Onani, nizakutumizilani chimanga, vinyu yasopano, na mafuta. Muzakutula navo, ndipo sinizaleka futi kuti munkale otukaniwa pa maziko. ²⁰ Nizakuchoselani ba chiwembu baku mpoto, naku bapishila mumalo yo yuma nayo taiwa. Bosogolela gulu yao ba enda ku nyanja ili kumawa, ndipo bakumbuyo kunyanja ili kumazulo. Kafungo kasanveka, naku nunka kwake koipa kusanveka." Zoon, achita vintu vikulu. ²¹ Musayope, imwe malo; nkala okondwela nao sangalala, chifukwa Yehova azachita vintu vikulu. ²² Musayope, imwe nyama zamusanga! Chifukwa vakudya vamu chipululu vizamela, mitengo izabala vipaso vake, mitengo yavi buyu naya mipesa izankala navipaso konse. ²³ Nkalani okondwela, imwe bantu bamu ziyoni, naku nkala osangalala muli Yehova Mulungu wanu. Pakuti azakupasani nvula yapachiyambi pantawi yake naku kugweselani nvula yambili, nvula yapachiyambi nanvula yoyambilila kugwa ntawi ya nvula. ²⁴ Popepetela paza zula na tiligu, navi gubu vikulu viza zula nama futa yasopano. ²⁵ "Nizakubwezelani zaka zavishango zamene gulu zantete zinadya_ ntete zikulu, ntete zenze kudya, nazenzele ku oononga_ gulu yanga yampanvu yamene nina kutimizilani. ²⁶ Muzadya vambili nakukuta, nakuyamika zina ya Yehova Mulungu wanu, wamene achita vodabwisa pali imwe, ndipo sinizakaletako futi manyazi pa bantu banga. ²⁷ Muzaziba kuti nili pakati pa Israeli, nakuti ndine Yehova Mulungu wanu, kulibe winangu, ndipo sinizakaletako futi manyazi pa bantu banga. ²⁸ Vikapita ivi pasogolo pake niza tumiza muzimu wanga pa bantu bonse, ndipo bana banu bamuna na bakazi baza nanenela. bamuna bakulu bazalota maloto; banyamata banu vazaona menso penya. ²⁹ Pali bakapolo bamuna naba kazi napeve, mumasiku ayo niza tumiza muzimu wanga. ³⁰ Nizalingiza vodabwisa kumwamba napa ziko lapansi, magari, mulilo, nachusi tolo. ³¹ Zuba izasanduka mudima na mwezi uzasanduka magari, ikalibe kubwela siku ikulu ya Yehova. ³² Chizankala kuti aliyense wamene aitana zina ya Yehova aza pulumusiwa. Pakuti pa pili ya Ziyoni mu Jerusalemu ndiye kuzankala abo bazakataba, monga Yehova anakambila, napa bo pulumuka, bamene Yehova aitana.

Chapter 3

¹ Onani, muma siku yaja napa ntawi ija, nikaenda kubaleta bamene bana patikiziwa kuchoka muziko ya Juda na Jerusalemu, ² Nizasonkanisa maziko yonse, naku yaleta ku chigwa cha Jehoshaphati. kuja kwamene niza baweluza, chifukwa cha bantu banga na cholowa changa Isiraeli, wamene bana mwaza pa ma ziko, na chifukwa kuti bana gabanisa malo yanga. ³ Bana chitila maela bantu banga, bana gulisa mwamuna kuvauule, naku kugulisa mukazi mwaku muchinjanisa na vinyu kuti bamwe. ⁴ Manje, nichani mwani kwiila, Tyrei, Sidoni na vigawo vonse vamu Philistiya? nanga muzani bwezela? Olo kuti muni bwezela, niza kubwezelani chilango pa mitu zanu mwamusanga. ⁵ Pakuti muna tenga siliva na golide yanga, nakungenesa vintu vanga vabwino muma kachisi yanu. ⁶ Muna gulisa bantu bamu Juda na Jerusalemu ku ma Greekisi, kuti chabe muba peleke kutali na malo yao. ⁷ v 7 Onani, nifuna kuba usha, kuchokela mumalo yamene muna bagulisamo, naku bwezela chilango chao pamutu panu. ⁸ Niza gulisa bana banu bamuna naba kazi, mumanja yabantu ba Juda. Nabo baza ba gulisa kulima Sabeansi, kuziko yakutali, chifukwa Yehova akamba." ⁹ Lalikilani ichi pama ziko: "Muzikonzekele va nkondo; ushani bazi muna bampantu; lekani babwele pa fupi; lekani bonse bazimuna bankondo babwele. ¹⁰ Pangani makasu yanu yankale malupanga na mipeni zojubila kunkala mikondo. lekani balibe mpanvu bakambe kuti, nili nampantu. ¹¹ Bwelani mwamu musanga, imwe bonse bamu maziko yapa fupi; mukasonkane pamozi kwamene kuja. Yehova, Gwesani pansi ba mpanvu banu. ¹² Lekani maziko yazi yazikonzekele yeka na kubwela ku chigwa cha Jehoshaphati. Pakuti kuja ndiye kwamene nizankala nakuweluza maziko yozungulila yonse. ¹³ Fakani muzenga, pakuti vokolola vanya. Bwelani, pwanyani mpesa, pakuti vopwanyilamo vazula. Vopwanyilamo vitaikila, chifukwa voipa vao nivambili." ¹⁴ Kuli pokoso, pokoso mu chigwa cha chiweluzo. chifukwa siku ya Yehova ilipa fupi muchigwa chachi weluzo. ¹⁵ Zuba na mwezi vankala mudima, nyenyezi zachepesa kuwala kwake. ¹⁶ Yehova azauluma kuchokela mu Ziyoni, naku kweza liu yake mu Jerusalemu. Kumwamba napansi kuzanyanganya, koma Yehova azankala chobisamilamo cha bantu, na linga yabantu ba Isiraeli. Mwaicho muzaziba kuti ndine Yehova Mulungu wanu wamene ankala mu Ziyoni, pili yanga yoyela. ¹⁷ "Pamene apo Jerusalemu izankala yoyela, ndipo kulibe bankondo bazapitamo futi. ¹⁸ Chiza chitika kuti pasiku ija mapili yaza chosa vinyu yabwino, pavitunda pazataikila mukaka, misinje yonse yamu Juda izataikiliwa na manzi, na kasupe iza chokela munyumba ya Yehova naku tilaila chigwa cha Shittimu. ¹⁹ Eygiputo izankala yosiiwa nakuonongeka, ndipo Edomu izankala chipululu chosiiwa, chifukwa chachiwawa china chitiwa kubantu bamu Juda, chifukwa bana tiila magari yabantu balibe mulandu mu malo mwao. ²⁰ Koma Juda azankala muyayaya, ndipo Jerusalemu izankala kuchokela mibadwo ku mibadwo. ²¹ Nizabwezela magari yao yamene nikalibe kubwezela, pakuti Yehova ankala mu Ziyoni."

Obadiah

Chapter 1

¹ Mpenya maso ya Obadiya. Ambuye Yehova bakamba ichi pali Idomu: Tamvela utenga kuchokela kuli Yehova koma nafuti mutumiki anatumiwa ku maiko, kukamba kuti, "Ima! Tiyeni ti imile kumenya naye nkondo!" ² Onani, Ine nizakulangani kunkala bochepekela pa maiko yonse; muzankala bosuliwa. ³ Kuzitukumula kwa mumutima mwako mwakuna boza, iwe wamene unkala pa kati pa myala, mu nyumba yako yapamwamba; wamene ukamba mumutima wako kuti, "Nanga kansi nindani wamene anganigwese pansi ine?" ⁴ Ungankale kuti wazikwezeka kumwamba monga, Ine nizakubwezela pansi kukuchosa pamwamba, akamba Yehova. ⁵ Ngati bakawalala bakuyendela iwe, ngati vigabenga vakubwelela usiku-ona mwamene uzaonongekelewa!-nanga kansi siba zaba chabe monga mwamene bafunila? ⁶ Mwamene Isau anaonongekelewa, chuma chake chobisika chabewa! ⁷ Bazibambo bonse bamene uli nabo na pangano bazakupilikisha kuyenda kumalile kwa ziko. Bamuna bamene banali na mutendere na iwe bakunama boza, nafuti baku gonjeza iwe. Baja bamene bamadya mukate wako baku ikila musampa pansi pako. Muli kusaziba mukati mwake. ⁸ "Kansi nanga ine sinizaka chita pa siku ija," Akamba Yehova, "Ononga bamuna banzeli mu Idomu na boziba kuchoka mu pili ya Isau? ⁹ Bamuna bako ba mpavu bazadabwa, Temani, mwakuti mwamuna ali onse aza onongeka mu pili ya Isau chifukwa cha kupaiwa. ¹⁰ Chifukwa cha voipa vamene vachitikiliwa mu bale wako Yakobo, iwe uzagwiliwa na manyazi, uzaonongeka muyayaya. ¹¹ Pa siku yamene unaimilila kosatandizila, pa siku yamene bantu bakunja banangena mu visoko vake, naku bejela Yelusalemu, iwe unali monga umozi pali beve. ¹² Koma usazitukumule chifukwa cha siku ya

mubale wako, pa siku yamene mavuto yamugwela, futi usakondwele pali bantu ba ku Yuda pa siku yabo yo onongeka; osazitukumule pa siku yabo yo onongeka. ¹³ Osangene mu chiseko pa siku yabo yo onongeka; osazitukumule pa siku yabo ya soka, osatenga chuma chabo pa siku yabo yo onongeka. ¹⁴ Osaimilila pakati pa njila kuti uononge bantu botaba, nafuti usa peleke bamene bapulumuka mu siku yotaya chiyembekezo. ¹⁵ Chifukwa siku ya Yehova ili pafupu ku maziku yonse. Monga mwamene wachitila, bazakuchitila iwe; zinthito zako zizakubwelela iwe pa mutu wako. ¹⁶ Monga mwamene iwe wamwelela pa pili yanga yoyela, ndiye mwamene maiko yonse yazamwela mosalekezela. Bazamwa naku mela monga siyanaliko. ¹⁷ Koma ku pili ya Ziyoni kuzankala baja bamene banapulumuka ndipo izankala yoyela; na nyumba ya Yakobo izatenga chuma chabo. ¹⁸ Nyumba ya Yakobo izankala mulilo, na nyumba ya Yosefe mulilo, na nyumba ya Isau izankala mauzu, ndipo bazaba ocha, nakubasiliza. Sikuzankala bopulumuka mu nyumba ya Isau, chifukwa Yehova akamba ichi." ¹⁹ Bantu bochokela ku Negevu bazatenga pili ya Isau na bantu ba mumalo ya pansi bazatenga malo ya a Filisiti. Bazatenga malo ya Efulemu na malo ya Samaliya, na Benjamini azatenga Giliyadi. ²⁰ Basilikali ba iyi gulu ya bantu ba Izilayeli bazatenga malo ya Kenani mpaka kukafikila ku Zalepati. Botaba mu Yelusalemu, bamene bali mu Sepaladi, bazatenga mizinda yaku Negevu. ²¹ Bopulumusa baza enda ku pili ya Ziyoni kukalamulila ziko yapa chulu ya Isau, na ufumu uzankala wa Yehova.

Jonah

Chapter 1

¹ 1 manje mau ya Yehova yanabwela kuli yona mwana mwamuna wa amitai, kukamba ati, ² "nyamuka na kuyenda ku Ninive, uja muzinda ukulu, na kukabazuzula, chifukwa voipa vabo vanyamukila pa menso panga." ³ koma yona ana nyamuka kutaba kuchoka pamenso pa Yehova na kuyenda ku tashishi. anayenda kusondomokela ku yopa na kupeza chombo choyenda ku tashishi. mwa ichi analipila mutengo na kukwela chombo kuyenda na beve ku tashishi, kuchoka pamenso pa Yehova. ⁴ koma YEHOVA anatuma chimpepo pa nyanja ndipo chinankala chimpepoi cha mpamvu pa nyanja. musanga musanga kuna oneka kuti chombo chiza ng'ambika. ⁵ ndipo bo chapa bana bwela bayopa maningi ndipo ali yense muntu ana punda kulila mulungu wake. bana ponya katundu wamu chombo mu nyanja kuchi pepusako. koma yona enze ana yenda pansi mumalo ya mukati mwa chombo.ndipo enze gone mutulo toyendelela. ⁶ 6 ndipo wo yanganila wao anabwela kuli eve nakukamba kuli eve, "uchita chani kugona? Nyamuka! itana mulungu wako! kapena mulungu azati yangana ndipo sitiza onongeka ." ⁷ Bonse bana kambisana, "bwelani, tichite mayele kuti tizibe wamene alengesa voipa ivi kuti vitichitikile. "ndipo bana chita mayele, na mayele yana gwela pali yona. ⁸ ⁹ ¹⁰ 8 ndipo bana kamba kuli yona, "tapapata ti uze nindani wamene alengesa voipa ivi vamene vitichitikila. usebenza nchito bwanji, ndipo una chokela kut?" ⁹ yona anakamba kuli beve, "ndine mu heberi; ndipo niyopa YEHOVA, MULUNGU wa kumwamba, wamene anapanga nyanja na ntaka yo yuma." 10ndipo ba muna bana nvelelatu manta na kukamba kuli yona, "nichani ichi chamene wachita?"popeza bamuna banaziba kuti enzo taba pa menso pa YEHOVA, chifukwa enze ana ba uza. ¹¹ ¹² ¹³ 11 ndipo bana kamba kuli yona, "tikuchite chani kuti nyanja yitinkazikikile?" popeza nyanja yenze kungo kalipilako. 12 yona anakamba kuli beve, "ninyamuleni na kuniponya mukati mwa nyanja. ndipoi nyanja izakunkazikilani, pakuti nizina kuti nichifukwa cha ine kuti chimpepo chikulu ichi chikuchitikilani." 13palibe vuto, amuna bana chapa mwa mpamvu kuti babwelele ku ntaka, koma sibana kwanise chifukwa nyanja yenze kungo yikilako ukali kuli beve. ¹⁴ ¹⁵ ¹⁶ mwa ichi bana lila kuli YEHOVA na kukamba. "tikupempani, YEHOVA, tikupempani, musatileke kuti ti onongeke chifukwa cha moyo wa uyu muntu, ndiponso musa ike pali ise mulandu wa imfa yake, chifukwa imwe YEHOVA , mwachita monga mwamene chakukondelesani." 15ndipo bana nyamula yona na kumuponya mukati mwa nyanja, na nyanja yina zizila. 16 ndipo bamuna bana yopa YEHOVA maningi. bana peleka nsembe kuli YEHOVA na kulumbila. ¹⁷ 17 manje YEHOVA ana konzekela chi nsomba chikulu chomela yona, ndipo yona anali mumimba mwa nsomba masiku yatatu na usiku utatu.

Chapter 2

^{1 2} 1 ndipo yona anapempela kuli YEHOVA MULUNGU wake mumimba ya nsomba. 2anakamba, "nina itana YEHOVA pa vuto yanga ndipo ana niyanka; kuchokela mumimba mwa nsomba nina lilila tandizo! munamvela liu yanga. ^{3 4} 3 mwenze munani ponya mukati pansi, mukati mwa mutima wa nyanja, na chimpepo chinani zunguluka; ----- . 4ninakamba.' na pishiwa kuchosewa pa manso panu; koma futi niza yangana kufupi na tempele yanu yoyela.' ^{5 6} 5manzi yana nivalila mukosi wanga wonse; kuzama konse kunani zunguluka; mauzu yamu nyanja ya nani pomba mutu. 6nina yenda kunyansi nyansi kwa ma pili; ziko na vi nsimbi vake vinani valililatu. koma muna leta moyo wanga kuuchosa muchi mugodi, YEHOVA, MULUNGU wanga! ^{7 8} 7pamene moyo wanga unakomoka mukati mwanga, nina itana YEHOVA kumaganiza; ndipo pempelo yanga ina bwela kuli imwe, ku tempele yanu yo yela. 8ba ika nzelu ku ku tumilungu tulibe pindu pamene batailila kukulupilika kwa pangano. ^{9 10} 9 koma kuli ine, nizapeleka nsembe kuli imwe na liu yo kamba zikomo; niza fikiliza vamene nalumbila. chipulumuso chichokela kuli YEHOVA!" 10 ndipo YEHOVA anakamba na nsomba, ndipo inaluka yona pa ntaka yo yuma.

Chapter 3

^{1 2 3} 1 mau ya YEHOVA yana bwela kuli yona ka chibili, kukamba, 2" nyamuka,yenda ku ninive, uja muzinda ukulu, ukaulalikile mau yamene nakulamulila kuti uwupase." 3ndipo yona ana nyamuka na kuyenda ku ninive, kulingana na mau ya YEHOVA. manje ninive unali muzinda ukulu, umozi waulendo wamasiku ya tatu. ^{4 5} 4 yona anayamba ku ngena mu muzinda pambuyo pa ulendo wa siku yimozi ana yitana na kukamba, "mumasiku 40 ninive aza gwezewa." 5bantu ba ninive bana kulupilila mulungu na kulamulila kusala kudya. boonse bana vala masaka, kuyambila bakulu na ba bafana bonse. ^{6 7} 6 musanga musanga mau yana fika kuli mfumu yaku ninive. ananyamuka pa mupando wake wa ufumu, nakuchosa mukanjo wake, kuzivininkila masaka, na kunkala mumilota. 7anatumiza mau yokamba kuti, "mu ninive, pa ulamulilo wa mfumu na bakulu bakulu ba mumuzinda: 'musaleke muntu aliyense olo nyama, kapena vibeto vili vonse, kulaba chili chonse. basadye, olo kumwa manzi. ^{8 9} 8 koma lekani bonse muntu na nyama bazivininkile na masaka ndipo mubaleke balile mo kuwa kuli mulungu. lekani aliyense atembenuke kuchoka ku njila zake zoyipa na ndewo ili mumanja mwake. 9nindani aziba? MULUNGU anga leke na kuchinja maganizo yake na kuchokako ku mukwiyo wake kuti tisa onongeke,'" ¹⁰ 10MULUNGU anaona vamene banachita, ndipo bana tembenuka kuchoka kunjila nzao zoyipa. mwa ichi MULUNGU anachinja maganizo yake pa chilango chamene enze anakamba kuti aza chita kuli beve, ndipo sana chite.

Chapter 4

^{1 2 3} 1 koma ichi yona sana kondwele nacho ana kalipa maningi. 2ndipo yona ana pempela kuli YEHOVA na kukamba, "ah,YEHOVA, sindiye ivi vamene nina kamba pamene nenze nikali ku ziko yanga? ndiye chifukwa chake nina yambilila na kuyesa ku taba kuyenda ku tashishi-chifukwa ninaziba kuti ndimwe MULUNGU wa mutima wabwino,wa chifundo,wosakalipa musanga ndiponso chikondi chanu ni chikulu, ndiponso mumazibweza ku kutuma chionongo. 3mwa ichi manje, YEHOVA, nikupempani, nipokeni moyo wanga, pakuti chiliko bwino kuti nife kuchila kunkala wa moyo." ^{4 5} 4 YEHOVA anakamba, "nanga nichabwino kuti wakalipa maningi?" 5ndipo yona ana choka mumu zinda nakunkala kumbali ya kumawa kwa muzinda. kwamene uko anazimangila tando nakunkala munyansi mwake muchimfwile kuti aone vamene viza chitika ku muzinda. ^{6 7} 6YEHOVA anapanga msatsi na ku ukulisa pamwamba pa yona kuti chinkale chimfwile pa mutu pake kuchepepako mavuto yake. yona anamvela bwino chifukwa cha msatsi. 7koma MULUNGU anakonza nyongolosi kuseneni seni. inaononga msatsi uja na msatsi una fota. ^{8 9} 8 inafika ntau pamene zuba ina choka kuseneni kokonkapo, MULUNGU anakonza mpepo yo kupya kuchoka kumawa. ndiponso, zuba inaseluka pa mutu pa yona ndiponso ana komoka. ndipo yona anafunisisa kuti amwalile. anazikambisa eka, "nkasako kuti nife kuchila kunkala wa moyo." 9ndipo MULUNGU anakamba kuli yona, "nanga nichabwino kuti wakalipa maningi pali msatsi?" ndipo yona anakamba, 'nichabwino kuti na kalipa, kochita kufa nako," ^{10 11} 10 YEHOVA anakamba, "wachitila msatsi chifundo wamene suna shange, wamene suna sebenzele, kapena ku ukulisa. unakula musiku imozi ndiponso unafa musiku imozi. mwa ichi kwa ine, sininga nkale na chifundo pali ninive, muzinda uja ukulu, mwamene muli bantu kupitilila 120,000 bamene sibaziba ku siyana pali kwanja yabo ya kumazele na kwanja yabo ya manja, ndiposo na vinyama vambili?"

Micah

Chapter 1

¹ Aya ni mau ya YEHOVA yamene yanabwela kuli mika waku molesheti mumasiku ya yotamu,Ahazi,Hezekaya, mfumu yaku Yuda, yamene anaona pali Samalia na Yelusalemu. ^{2 3 4} 2 Nvelani, moonse imwe bantu. nvela ziko na voonse vili mukati mwa iwe. leka AMBUYE YEHOVA ankale mboni pali iwe, AMBUYE kuchoka pa tempele yake yoyela.3 yangana YEHOVA achoka mumalo yake; azaseluka pansi nakudyaka pamalo yapamwamba ya ziko ya pansi. 4 Mapili yazasungunukila pansi pake; vigwa vizapwanyikana, munga phula pamulilo, munga manzi yamene yatayiwa pansi posondoka. ⁵ Voonse ivi nichifukwa cha machimo ya yakobo, na chifukwa cha machimo ya nyumba ya isilayeli. nanga yakobo machimo yake nichani? nanga si samalia? malo ya pamwamba ya yuda ni chani? si yelusalema? ^{6 7} 7 samalia nizamupanga bwinja, munda wolimamo mpesa, ndipo nizatila myala zake mukati mwachigwa ndipo nizavununkula maziko yake. 7Vobeza beza vake voonse viza pwanyika mutuduswa duswa, na mpaso zake zoonse zamene analandila zizashokewa na mulilo, ndipo nizaononga tumafano twake toonse. pakuti ana unjika mpaso zake kuchokela kumalipilo yake ya uhule, yazankala futi malipilo ya mahule". ⁸ ^{9 10} 8 chifukwa cha ichi nizapunda nakulila; nizayenda nilibe nsapato na chintako; nizapunda munga nkandwe na kulila munga vinyoni. 9 pakuti vilonda vake sivipola, pakuti vabwela kuli yuda. vafika pavipata va bantu banga, kufika kuyelusalema. 10 musavikambepo mu Gati; musalile nakulila.pa Beti Lefula nizekunkulusa mudoti. ^{11 12} 11 Mupitile mumalo yabamu safere, muli chintako na manyazi. bonkala mu zanani sibachoka panja. Beti Ezel alila, pakuti kuchingiliziwa kwao kwa chosewapo. 12 pakuti bonkala mu maroti ba yembekezela utenga wabwino na nkawa, chifukwa chionongo chabwela pansi kuchokela kuli YEHOVA ku vipata va yelusalema. ^{13 14} 13 Mangani magaleta ku gulu ya akavalo, bonkala mu Lakisi. iwe, lakisi, munalu kuyamba kwa uchimo wa mwana wa ziyoni, pakuti muli iwe machimo ya isilayeli yanapezeka.14 mwa ichi uza pasa moreseti gati mpaso yo patukana; mizinda ya akizibi izafokesa mfumu zaku isilayeli. ^{15 16} 15 Nizakuletelani futi bokuchilani, imwe bonkala mu maresa; bakulu bakulu baku isilayeli bazabwela ku adulamu. 16 Gelani mitu zanu nakujuba sisi chifukwa cha bana bamene mukondwela nabo. muzipange bolimbika mitima munga viomba nkanga, chifukwa bana banu bazayenda chiyende yende.

Chapter 2

^{1 2} 1 Soka kuli abo bamene bakonzekela voyipa, kuli abo bamene bakonzekela pogona pao kuchita voipa. kuseni seni bavichita chifukwa bali na mpamvu. 2 bafunisisa minda na kuipoka; bafunisisa manyumba na kuyatenga. batitikiza muntu na nyumba yake, muntu na cholowa chake. ^{3 4 5} 3 Mwa ichi YEHOVA akamba ichi," yangana, nili pafupi nakuleta chi onongeko pa chi ongo ichi, pamene simuza chosa mikosi yanu. simuza yenda mozinvela, pakuti izankala ntau yoipa. 4 pasiku ija bantu bazayimba nyimbo pali iwe, na kulila ko punda. bazayimba, 'ise ba isilayeli ta onongekelatu; YEHOVA achinja malo ya bantu banga. anga yachose bwanji pali ine? agabanisa minda zatu kuli botigulisa!'" 5 mwa ichi imwe bantu bolemela muzasoba vizukulu vogabana malo yanu mu nyumba ya YEHOVA. ^{6 7 8} 6 "bakamba kuti," osanenela." basanenele ivi vintu; vovutisa visabwele." 7 nivofunikila kuti vikambiwe ayi, nyumba ya yakobo, "ninshi muzimu wa YEHOVA wakalipa? ivi nivochita vake zoona?" ndiye kuti mau yanga siyachita vabwino kuli ali yense wo yenda muchilungamo? 8 konse uku bantu banga banyamuka monga mudani. mun'gamba mikanjo, ya bopita chabe bakaye, pamene bankondo babwelera kuchokela kunkondo kuyenda kwamene baganiza kuti kuli bwino. ^{9 10 11} 9 muchosa bazimayi ba bantu banga mumanyumba yao yabwino; bana bao ban'gono mubapoka madaliso yanga kubapokelela. 10 nyamukani muchoke, pakuti aya simalo yamene mungankale, chifukwa chaku desedwa kwake; yana onongewa na chionongeko chosililatu. 11 ngati muntu winango abwela kuli imwe mumuzimu waboza nonama nokamba," niza nenela kuli imwe pa vinyo na vakumwa vikali," azatengewa kunkala muneneli wa bantu bake. ^{12 13} 12 Nizakusonkanisani moonse, yakobo. nizasonkanisa bosala ba isilayeli. nizababwelesa pamozi monga nkosa mukola, monga vobeta pakati pa mauzu yake. kuzankala chongo chikulu chifukwa cha kupaka kwa bantu. 13 winango wo basegulila njila azasogola. bapwanya vipata nakuchoka panja; mfumu yao izaba pitilila kusogolo kwao. YEHOVA aza gwililila kwanja yao.

Chapter 3

^{1 2 3} 1 Nina kamba, "manje mvelani, imwe basogoleli ba yakobo na bolamulila ba nyumba ya isilayeli: sichabwino kuli imwe kumvesesa chilungamo? 2 imwe bamene muzonda vabwino na kukonda voipa, imwe bamene mung'amba nkanda yao nyama yao kumafupa yao- 3 imwe bamene mumadya nyama ya bantu banga, na kung'amba nkanda yao, kupwanya mafupa yao, na kubajuba mutuduswa duswa, monga nyama yoika mupoto, monga nyama mopikila. ⁴ 4 ndipo imwe bolamulila muzalila kuli YEHOVA, koma saza kuyankani. Azabisa pa menso pake kuli imwe pantawi yamene iyo, chifukwa mwachita vonyansa." ^{5 6 7} 5 YEHOVA akamba ichi, "ngati nibaneneli bamene banasobesa bantu banga, ngati winango aba pasa chakudya, bakamba, 'mutendele.' koma ngati sana yike chintu mukamwa mwao, bazipeleka ku usha nkondo pali eve. 6 mwa ichi, uzakunkalilani usiku ulibe manso mpenya; kuzafipa kwakuti simuzakwanisa no bwebweta. zuba izaba mbilila baneneli, nasiku izabafipila. 7 ba neneli baza mvesewa manyazi, nabo bwebweta baza sokonezeka. boonse baza vala milomo zao, pakuti kulibe yanko kuchokela kuli ine." ⁸ 8 koma kuli ine, ndine ozula mpamvu na muzimu wa YEHOVA, ndipo ndine ozula chilungamo na mpamvu, kukamba kuli yakobo voipa vake, na kuli isilayeli uchimo wake. ^{9 10 11} 9 manje nvelani kuli ichi, imwe basogoleli ba nyumba ya yakobo, na bolamulila ba nyumba ya isilayeli, imwe bamene munyansiwa na chilungamo, na kupotoloza voonse chabwino. 10 mumanga ziyoni na magari na yelusalema na uchimo. 11 basogoleli banu bafuna ku woshewa, ba nsembe banu bapunzisa na malipilo, na baneneli banu ba bwebwetela ndalama. futi muchetekela pali YEHOVA na kukamba, "si YEHOVA ali na ise? kulibe choipa chizabwela pali ise." ¹² 12 mwa ichi, chifukwa cha iwe, ziyoni azankala munda wolimiwa, yelusalema azankala bwinja, na chulu chatempele chizankala nkhalango.

Chapter 4

¹ koma mumasiku yosiliza yazapezeka kuti pili ya nyumba ya YEHOVA iza konzewa bwino kuchila mapili yenango. izanyamuliwa pamwamba pa machulu, na magulu yabantu yaza tamangila kuli eve. ^{2 3} 2 maiko yambili yazayenda nokamba kuti. "bwelani, tiyeni tiyende pamwamba papili ya YEHOVA, ku nyumba ya mulungu wa yakobo. azati punzisa njila zake, ndipo tiza yenda mwamene apita. "pakuti mu ziyoni lamulo izachokamo, na mau ya YEHOVA kuchoka mu yelusalema. 3 azaweluza pakati pa bantu bambili ndipo azasanka pa mayiko yambili mbili yakutali. bazapwanya malupanga yao kuya sandusa vo gaulila na mikondo yao kuyipanga mapwitika. ziko siyiza nyamula lupanga kunyamulila ziko inzake, olo kukonzekela futi nkondo. ^{4 5} 4 koma, bazankala aliyense muntu pansi pa munda na pansi pa mutengo wake wa mpesa. kulibe wamene aza bayofya, pakuti kamwa ya YEHOVA wa makamu ya kamba. 5 pakuti bonse bantu bayenda, aliyense. muzina ya mulungu wake. koma tizayenda muzina ya YEHOVA MULUNGU watu kwa muyayaya. ^{6 7 8} 6 "pasiku ija"-uku nikukamba kwa YEHOVA -"niza sonkanisa pamozi bolemala na ku unjika ba kunja, abo bamene nina vutisa. 7 niza chinja bolemala kuba panga bosalako, na bopishiwa kunkala ziko yolimba, ndipo ine YEHOVA , niza ba lamulila pa pili ya ziyoni, manje na muyayaya, 8 koma kuli iwe wo yanganila vi beto, chulu cha mwana mukazi wa ziyoni-kuli iwe chiza bwela, ulamulilo wako wakudala uzabwezewa, ufumu wa bana bakazi ba ku yelusalema. ^{9 10} 9 manje, chifukwa chani upunda maningi? ninshi pungu wako amwalila? ninshi ndiye chifukwa chake kubaba kukugwila monga muzimai ali mukubala? 10 nvela kubaba nakusebenza nampamvu kuti ubale, mwana mukazi wa ziyoni, monga muzimai ali mukubala. pali manje uzayenda kuchoka mumuzinda, kunkala mumunda, na kuyenda ku babiloni. kweve baza ku pulumusa. kweve YEHOVA aza ku pulumusa kuchoka mu kwanja kwa badani bako. ^{11 12} 11 manje ma yiko yambili yasonkanila iwe; bakamba, 'lekani adesedwe; lekani menso yatu yamvele bwino pali ziyoni.' 12 sibaziba maganizo ya YEHOVA , kapena kumvesesa kukonzekela kwake, pakuti aba unjika monga mitolo ya tirigu yamene yakonzekelwa kupuntiwa. ¹³ 13 nyamuka na kumpunta, mwana mukazi wa ziyoni, nizapanga nyanga yako kunkala nsimbi, nizapanga----- uza pwanya bantu bambili ndipo uza peleka chuma chao chosalungama kuli YEHOVA, chuma chao kuli MBUYE wa ziko lonse lapansi."

Chapter 5

¹ 1 manje bwelani pamozi muntepe za nkondo, mwana mukazi wa ba silikali! batizunguluka ba nkondo! na ndodo ba menya wo weluza wa isilayeli pa mbovu. ^{2 3} 2 koma iwe, betelehemu efurata, olo ndiwe mung'ono pakati pa mitundu ya yuda, muli iwe umozi azbwela kuli ine kuti alamulile mu isilayeli, wamene kuyamba kwake nikwa ntau ya kudala, kuchoka muyayaya. 3 mwa ichi MULUNGU aza ba peleka, kufika ntau yamene eve ali mu kubaba ko bala abale mwana, na boonse bakulu bake ba muna babwelele ku bantu ba isilayeli. ^{4 5} 4 Aza nyamuka na kubeta vi beto vake mumpamvu za YEHOVA, mu ulemelelo wa zina ya YEHOVA MULUNGU wake. bazasala, pali iyo ntau aza nkala mukulu mpaka kusila kwa ziko lapansi. 5 popeza ndiye uza nkala mutendele-ngati basiliya babwela muziko yatu, ngati babwela kuti tila nkondo, tiza ba nyamulila bazibusa 7 na basogoleli 8 pa bamuna. ^{6 7} 6 baza beta ziko ya asiliya na panga, na ziko ya nimurodi mu vipata vake. aza tipulumusa kuli a siliya, bakabwela muziko yatu, baka bwela mukati mwa malile yatu. 7 bosalako ba yakobo bazankala pakati pa bantu bambili, monga mame kuchokela kuli YEHOVA, monga tumvula towaza pa mauzu, yamene siya yembekeza muntu, ndipo siya yembekeza bana ba muntu. ^{8 9} 8 bosalako ba yakobo bazankala pakati pa mayiko, pakati pa bantu bambili, monga nkalamu pakati pa nyama za musanga, monga kamwana ka nkalamu pakati pa vibeto va nkosa. akayenda pakati pa veve, aza vidyaka dyaka na kuvi ng'amba mu tu duswa duswa, ndipo kuzankala kulibe wo vi pulumusa. 9 kwanja yako iza nyamuliwa pali badani bako, na kuba ononga. ^{10 11} 10 "viza chitika pasiku ija"-uku ni kukamba kwa YEHOVA-"kuti niza ononga ba kavalo banu kuchoka pakati panu na ku bongoshola ma magaleta yanu. 11 niza ononga mizinda mu ziko yanu na kugwesa vipupa vanu. ^{12 13 14 15} 12 niza ononga umfwiti mumanja mwanu, ndipo muzankala mulibe futi bo bwebweta bali bonse. 13 niza ononga mafano yanu na sandamila zanu za myala kuchoka pakati panu. simuza pembeza futi vobeza va manja yanu. 14 niza nyula mitengo ya mikula kuchoka pakati panu, ndipo niza ononga mizinda yanu. 15 niza chita bwezela mu ukali na mkwiyo pa mayiko yamene siyana nvele."

Chapter 6

^{1 2} 1 manje nvela kuli vamene YEHOVA akamba." nyamuka na kupeleka mulandu wako pamenso pa mapili; leka vyulu vinvele liu yako. 2 nvela ku mulandu wa YEHOVA , iwe mapili, na iwe maziko yopilila ya ziko yapansi. pakuti YEHOVA ali nawo mulandu na bantu bake, ndipo aza menya nkondo mubwalo ya milandu pali isilayeli." ³ ^{4 5} 3 "bantu banga, nichani chamene nachita kuli imwe? na kudesani nkaba munjila bwanji? nichitileni umboni! 4 pakuti nina kuchosani muziko ya ejipito na kuku pulumusani kuku chosani munyumba yo mangiwa. nina tuma mose, Aaron, na mirriam kuli imwe. 5 bantu banga, kumbukilani vamene balaki mfumu ya ku mohabu yenzo funa kuku chitani na mwamene balamu mwana mwamuna wa beori anamuyankila pamene mwenze kuchoka ku shitimu kuyenda ku giligala, kuti muzibe vochita va YEHOVA volungama." ^{6 7 8} 6 Nichani chamene nizaleta kuli YEHOVA, pamene nigwada pansu kuli MULUNGU wa pa mwamba? kodi nibwele kuli eve na chopeleka cho fukiza, na tubana twa ng'ombe twa chaka chimozi? 7 kodi YEHOVA azakondwela nato tubana twa nkosa ma sausande, olo na 10 sausande ya tumumana twa mafuta? kodi nipeleke mwana wanga woyamba pa machimo yamo, chipaso cha tupi yanga pa machimo yanga neka? 8 aku uza, muntu, nichani chabwino, ndipo chamene YEHOVA afuna kuli iwe: chita chilungamo, chikondi chabwino, nakuyenda mozi chepesa na MULUNGU wako. ^{9 10} 9 ni liwu ya YEHOVA ipanga chi zibiso ku muzinda- nga nkale manje nzelu iziba zina YANU: "faka nzelu ku ndodo, nakuli wamene ayi ika mu malo. 10 muli chuma muma nyumba yaboipa chamene chilibe chilungamo, na mipimo ya boza yo desedwa. ^{11 12} 11 nilekelele muntu kunkala alibe mulandu koma asebenzesa sikelo yo bela, na chola chili na mipimo za boza? 12 bantu bolemela nibo zula na ndeo, bonkalamo bakamba ma boza, na lilime yao mukamwa mwao niya chinyengo. ^{13 14 15} 13 mwa ichi niza kukantani moyipisisa, ndipo niza kupangani malo yo siyiwa chifukwa cha machimo yanu. 14 muzadya koma simuza kuta; muzankalilila mulibe chintu mukati mwako. muzasunga katundu koma siiza sungika, na vamene musunga niza pasa mukondo. 15 muza shanga koma simuza kolola; muza pwanja olivi koma simuza zizoleka na mafuta; muza fina mpesa koma simuzamwa vinyo. ¹⁶ 16 malamulo yana pangiwa na omuri mwasunga, na vo chita voonse va nyumba ya ahabu. muyenda kulingana na malangizo awo. mwa ichi niza kupangani, muzinda, wo onongeka, na bantu ba mitundu baza kunyodolani, ndipo muza nyamula manyozo ya bantu banga."

Chapter 7

^{1 2} 1 wasoka ndine! nankala monga vipaso va ntau ya zuba, ndiponso monga mpesa za kololewa; kulibe mpesa zosalako zokudya, kulibe mukuyu wokupya musanga wamene moyo wanga ukumbwila. 2 bokulupilika ba soba kuchoka pa ntaka; kulibe muntu olungama mu umuntu onse. boonse bayembekezela kutaya magari; aliyense asakila sakila mubale wake na sumbu. ^{3 4} 3 manja yabo yaziba bwino kupweteka: bolamulila bafuna ndalama, boweluza nibokonzekela ku woshewa, ndiponso muntu wa mpamvu auza benangu vamene afuna kupeza. mwa ichi ba pangana pamozi. 4 wabwino maningi pa bonse ali monga lunguzi, wolungama pa bonse achila na kosilizila kwa minga. ni siku yamene ina kambiliwatu na bokulondani, siku ya chilango chanu. manje ni ntau ya musokonezo wao. ^{5 6} 5 osa chetekela ali yense wamene munkala naye pa fupi; usankale na kuzinvela mumunzako ali yense. uchenjele pa vamene ukamba olo kuli mukazi wamene agona mumanja mwako. 6 pakuti mwana mwamuna samvelela atate, mwana mukazi mupongozi aukila apozi bake. badani ba muntu ni bantu ba munyumba mwake. ^{7 8} 7 koma kuli ine, nizayangana kuli YEHOVA . niza yembekezela MULUNGU wa chipulumuso changa; MULUNGU wanga aza nimvela. 8 musasangalale pali ine. nikagwa, niza nyamuka. nikankala mumudima, YEHOVA azankala nyali yanga. ⁹ 9 chifukwa nina muchimwila MULUNGU wanga, niza pilila ukali wake mpaka animvelele chifundo, na kuchita chiweluzo pali ine. azanibwelesa ku nyali, ndipo niza muona anipulumusa muchi lungamo chake. ¹⁰ 10 ndipo badani banga baza chiona, na manyazi yaza vininkila wamene anakamba kuli ine, "alikuti YEHOVA MULUNGU wako?" menso yanga yaza muyangana; aza dyakiwa dyakiwa monga matika mu njila. ^{11 12 13} 11 siku yomanga vipupa vako yiza bwela; pa siku ija malile yaza fendezeza kutali maningi. 12 pasiku ija bantu bako bazabwela kuli miwe, kuchokela ku asiliya na kumizinda za ku ejipito, kuchoka ku ejipito kuyenda ku mumana, kuchoka ku nyanja kuyenda ku nyanja, ndiponso kuchokela kupili kuyenda ku pili. 13 koma malo yazankala yo siyiwa chifukwa cha bantu bamene bankalamo, chifukwa cha vipaso va chinto zao. ¹⁴ 14 beta bantu bako na ndodo yako, vi beto va choloba chako. bankala beka mukalango, pakati pa mauzu ya bwino. baleke badye mu bashani na giliadi monga masiku ya kudala. 15 monga mumasiku yamene munachoka mu ziko ya ejipito, niza balangiza vodabwisa. ^{16 17} 16 ma yiko ya zaona na kumvela manyazi pa pamvu zao zoonse. baza yika manja yabo pa kamwa pao; matu yao yazaleka kumvela. 17 baza myanguta doti monga njoka, monga volengewa vo kwaba pa ziko ya pansi. bazchoka mu migodi nyao na manta; baza bwela kuli imwe na manta, YEHOVA MULUNGU watu, ndipo baza nkala na manta chifukwa cha imwe. ¹⁸ 18 nindani MULUNGU monga imwe-wamene achosa machimo, wamene ayibala volakwa va bosalapo ba choloba chake? sa sungilila ukali wake kwa muyayaya, chifukwa asangalala muku kulupilika kwa pangano yake. ^{19 20} 19 muzatichitila futi chifundo; muza dyaka dyaka voipa watu pansi pa mendo yano. muza taya machimo yatu yoonse pansi pa nyanja. 20 muza pasa cha zoonza kuli yakobo na kukulupilika kwa pangano kuli abulamu, mwamene muna lumbila ku makolo yatu muma siku yakudala.

Nahum

Chapter 1

¹ Uthenga pali Nineve. Buku ya volembewa pali Nahumu, wa mutundu wa Elikoshite. ² Yehovah ni Mulungu wa nsanje wamene amabwezela; Yehovah amabwezela naukali wofikapo; Yehovah amabwezela badani bake, amapitilila nao ukali wake pali badani bake. ³ Yehovah amachedwa kukalipa komafuti niwa mpavu zambili; sazavomeleza kuti bantu boipa baende kopanda kulangiwa. Yehova amapanga njila yake mwine mu kavuluvulu na mu chimpepo, na makumbi ndiye fuvu yaku mendo yake. ⁴ Amakalipila nyanja naku yiyumika; amayumika mimana zonse. Bashani alibe mpavu, na Kalamelo na eve; maluba yaku Lebanoni niyofota. ⁵ Malupili yama njenjema chifukwa cha kupezekapo kwake, zo ona, ziko na bantu bonse bamene bankalamo. ⁶ Nanga nindani wamene anga imilile ukale wake? Nanga nindani wamene angashushe ukale wake? Ukali wake umatiliwa monga mulilo, na myala zimapwanyika na eve. ⁷ Yehovah niwabwino, obisamilamo muntawi yama vuto; ndipo niwokulupilika kuli baja bamene bamazi chingilizila muli eve. ⁸ Koma azabasilizilatu badani bake na chigumula chikulu; azabapilikisha kufikila mu mufinzi. ⁹ Nanga imwe bantu kansi nivichani vamene muganzila Yehova? Azakwanilisa kuvisilizilatu; mavuto siyazabwelela kachibili. ¹⁰ Monga minga zopombana futi monga moba waba chakolwa, bazaonongeka monga mauzu yoyuma. ¹¹ Wina anaima pakati panu, Nineve, wamene ana lingilila voipa pali Yehova, muntu wamene anachulukisa voipa. ¹² Ichi ndiye chamene Yehovah akamba,

"Bangankale kuti bali bofikapo ku mpavu na kupendewa, koma bazaka-onongeka; bantu bazakasila. Koma iwe, Yuda: Nangu kuti nakuvutisa, sinizakuvutisa nafuti." ¹³ Apa manje nizatyola ngoli kuichosa pali iwe; nizapwanya ma bango yako." ¹⁴ Yehova apeleka lamulo pali iwe, Nineve: "Sikuzakankala mubadwe wamene uzakatenga zina yako. Nizachosapo mafano na mafano yansimbi mumanyumba ya milungu zako. Nizakumba manda yako, chifukwa ndiwe wonyansa." ¹⁵ Ona, pa mapili pali mendo ya muntu wamene aleta utenga wabwino, wamene aulusa mutendere! Sangalalani myambo, Yuda, nakusunga lonjezo, chifukwa oipa sazakuyendelani nafuti; aonongekelatu kosililatu.

Chapter 2

¹ Eve wamene amapasula akubwelela iwe. Londa chibumba cha muzinda, yanganila museu, konzekela nkondo, konzekela na mpavu zako zonse. ² Chifukwa Yehova abwezela ulemelelo wa Yakobo, monga na ulemelelo wa Izilayeli, ngakale kuti bo-ononga babaononga naku baonongela mitengo za vinyu. ³ Vochingilizila va bampavu bake vili vo chofiyira, na basilikali bavala vovala vofiyira; ma gareta yabeka chifukwa cha nsimbi zabo pa siku pamene yakonzewa, mikondo za saipulesi wazi imya mumwamba. ⁴ Ma gareta ya tamangisiwa mu miseu; yatamanga uku na uku mu miseu zikulu. Zioneka monga nyali, nakutamanga monga kaleza. ⁵ Wamene azakupwanyani mu vidunswa vidunswa aitana ba silikali bake; bagwelana pamene ba tamangila; batamangila kuti bagonjese chipupa cha muzinda. Chishango chikulu chikonzewa kuti chibachingilize aba bankondo. ⁶ Viseko vaku manzi vipwanyika, na nyumba ya mfumu ionongeka. ⁷ Huzabu avuliwa vovala vake nakutengewa; bantchito bake bakazi balila monga tunkunda, uku bazimenya pachifuba. ⁸ Nineve ili monga pali manzi, pamozi na bantu bake pamene bataba monga manzi yamene yakunkuluka. Benangu bapunda kuti, "Lekani, lekani," koma kulibe wamene alangana kumbuyo. ⁹ Tengani chuma cha siliva, tengani chuma cha golide, chifukwa kulibe kosilizila, ku ulemelelo wake wa Nineve mu vabwino. ¹⁰ Mu Nineve mulibe kali konse ndipo yaonongeka. Mitima za bonse zapwanyika, mabobndo ya muntu ali onse yamenyana, kukalipa mutima kuli muli ali onse; pa menso pabo ni pofoka. ¹¹ Kansi nanga monkala nkalamu nimuti, malo yamene tu bana twa nkalamu tunali kudyesewa, malo yamene nkalamu imuna na ikazi zinali kuyenda, pamozi na tubana twabo, nanga kunali vamene zinali kuyopako? ¹² Nkalamu inali kung'amba nyama zake mu vidunswa vidunswa kupasa bana bake, inali kuponyongola nyama zake kuchitila nkalamu zikazi zake, na kuzulisa monkala mwake na nyama, monkala mwake na nyama zakufa. ¹³ "Ona, Ine nishushanya naiwe-uku niku kamba kwa Yehova wa makamamu. Ine niza ocha ma gareta yako mu chusi, na mukondo wako uza ononga tunkalamu twako tubana. Nizachosamo nyama zakudya mu ziko yako, na liu ya batumiki si izakamvekako futi."

Chapter 3

¹ Soka ku muzinda wozula na magari! Niwozula na maboza na chuma chakuba; bobelewa bali mukati mwake ntawi zonse. ² Koma manje kuli chongo cha mikwapu na chongo cha kulila kwa mawilo ya garetu, mendo ya akavalo, na kubwela kwa garetu. ³ Kuli bankondo bali pa ma kavalo, uku balangiza mikondo, mipeni zamene zibeka, ma chulu ya bantu bakufa, machulu yakulu ya mitembo. Kulibe pamene mitembo zisilila; bomenyana nkondo nabo bagwelapo. ⁴ Ivi vichitika chifukwa cha vilako lako va wachiwelewele wabwino, kaswili mu umfwiti, wamene agulisa ma ziko kupitila mu uchiwelewele, na bantu bake kupitila mu nthito zake za umfwiti. ⁵ "Ona, Ine niku shusha iwe-uku ndiye kukamba kwa Yehova wa makamu-Ine niza imya chovala chako kufika pamenso pako naku langiza chintako chako ku maziko, manyazi yako ku ma ufumu yonse. ⁶ Nizataya vonyansa pali iwe naku kulenga kunkala wonyansa; Nizakulenga kunkala muntu wamene muntu ali onse azalanganapo. ⁷ Chizachitika mwakuti ali onse wamene azalanganapo pali iwe azakutaba naku kamba kuti, 'Nineve yaonongeka; nanga nindani wamene azamulila?' Kansi nikuti kwamene nizapeza wamene azakupuziika?" ⁸ Nineve, nanga kansi iwe ndiwe opambana kuchila Tebesi, yamene inamangiwa pa mumana wa Naile, wamene unali na manzi yoizungulila, unali kuchingilizwa na nyanja, ndipo nyanja yamene iyi inali chitetezo chake? ⁹ Kushi na Igupto banali mpavu zake, ndipo kunalibe kosilizila kuli eve, Puti na Libiya banali pamozi na eve. ¹⁰ Koma Tebesi anatengewa; anayenda mu ukapolo; bana bake bang'ono bana paiwa mopwanywa mitu pa mutu wa njila ili yonse; badani bake banali ku beja kufuna bantu bake bolemekezeka, bonse bamuna bakulu banali kumangiwa ma unyolo. ¹¹ Naiwe uzakolewa; uzafuna kubisama, nakufuna funa malo yobisamilamo kutaya badani bako. ¹² Monse mobisamilamo mwako muzankala monga mutengo wa mukuyu wamene uli na vipaso voyamba vokupya: ngati ba gwedezeka, bagwela mukamwa mwa uja wakudya. ¹³ Ona, bantu mukati mwako ni bakazi; viseko vaku ziko yako vaseguliwa kuli badani bako; mulilo waononga vokomelako. ¹⁴ Enda ukatape manzi kukonzekela nkondo; limbikisa mobisamamo; enda mu doti ukaumbe daka; tenga vopangilamo ma buloko. ¹⁵ Mulilo uzaku ononga iwe kuja, na lupenga uzaku ononga. Uzaononga iwe monga mwamene ntente zing'ono zima onongela vintu vonse. Zipakiseni pamweka monga tu ntete tung'ono, mupake monga ntente zikulu zikulu. ¹⁶ Mwapakisa bamalonda kuchila nyenyezi zaku mwamba; koma bali monga ntente zing'ono: baononga ziko naku mbululuka. ¹⁷ Bana ba mfumu nibambili kulingana na ntente zikulu zikulu, na bakulu bakulu ba nkondo bali monga gulu ya ntente yamene imankala pa vibumba pa siku ya mpepo. Koma pamene zuba ichoka vimbululuka kuyenda kumalo kwamene kulibe wamene aziba. ¹⁸ Mfumu yaku Asiliya, bokubetela baligone; basogoleli bali gone pansi bapumula. Bantu bako bataikana pa mapili, ndipo kulibe obabwezela pamozi. ¹⁹ kulibe kupola ku vilonda vako ivo. Vilonda vako nivikulu maningi. Muntu ali one wamene azamvela nkani iyi pali iwe azaombela manja mokondwela. Nanga nindani wamene anakwanisa kutaba kuipa kwako?

Habakkuk

Chapter 1

¹ Utenga wamene Habakuku muneneli analandila, ² "Yehova, nizalila kwantawi itali bwanji, mukalibe kuninvela? Nililila kuli imwe, 'Chiwawa!' koma simunani pulumuse. ³ Nichani mumaleka kuti nione uchimo naku langana pa vochita voipa? Chionongeko na chiwawa vili pamenso panga; kuli mukangano, nakuyambana kwanyamuka. ⁴ Mwaicho malamulo yapepusiwa, ndipo chiweluzo sichinkala pa ntawi ili yonse. pakuti boipa bazunguluka bolungama; mwaichi chiweluzo chaboza chichokelela. "Yehova anamuyanka Habakuku ⁵ "Langana ma ziko naku yayesa; nkala odabwa naku naku dawisiwa maningi! chifukwa nifuna kuchita chintu mumasiku yako chakuti suzakachikululupilila ukaenda ku chinvela. ⁶ Pakuti ona! Nifuna kunyamula ma Chaldeanis_ uja mutundu oyofya na wochela- baenda enda muziko yonse yamu munzi kupoka manyumba yamene siyanali yao. ⁷ Bayofya naku yopesa; chiweluzo na ulemelelo wao upitiliza kuchokela kuli bene bake. ⁸ Makavalo yao yamatanga manga maningi kuchila Nyalugwe, changu kuchila mimbulu yausiku. Mwaicho makavalo yao yapambana, naba pakavalo ba chokela kutali maningi- ba mbululuka monga nkwaizi wamene atamangila kudya. ⁹ Bonse bamabwelela nkanza; kupaka kwao kuli maenda monga chimpepo mu chipululu, ndipo bama sonkanisa bakapolo ngati michenga. footnote The copies of the ancient Hebrew text are translated here, "their multitudes go like the desert wind" ; this is a difficult passage to translate, and it is translated in different ways in modern translations. ¹⁰ Mwaicho bama nyoza manfumu, bolamulila balimonga choseka kuli beve. Bamaseka chitetezo

chili chonse, chifukwa bama faka pamozi ziko naku itenga.¹¹ Chokonkapo chimpepo chizapitapo; chizaenda musanga kupitilila- bantu bochimwa, abo bamene kupambana ndiye mulungu wao." Habakuku afunsa Yehova funso inangu¹² "Nanga sindimwe bamu ntawi yakudala, Yehova Mulungu wanga, Oyela wanga? Sitizafa. Yehova anabaika kuti ba weluza, naiwe, mwala,vankazikisiwa pa kulungamisiwa.¹³ Menso yako niyoyela maningi kuyangana pa choipa, ndipo sumkwanisa kulangana vochitika voipa na chisomo; Nichani kansi walangana nachisomo pali abo bamene baku pachikani? Nichani mwankalila zii koma boipa bamela abo bolungama kuchila beve?¹⁴ Mupanga muntu monga nsomba mu nyanja, monga vintu vokwawa vilibe ovilamulila.¹⁵ Ama leta vonse pamwamba na mbeza; naku faka bantu molobela nsomba; aba sonkanisa pamozi mumu koka wake; ndipo asangalala naku kondwela.¹⁶ Mwaichi apeleka nsembe ku ukonda wake naku shoka vonunkiliza ku mikoka yake, pakuti mumu konda wake ankala bwino, nava kudya vake nivija vamutundu wolemela.¹⁷ Nanga azapitiliza kuchosa vonse mu ukonda wake, nanga azapitiliza futi kucheka ma ziko kopanda chifundo?"

Chapter 2

¹ Nizaimilila pamalo yanga yolondela naku ziimilika pa linga, ndipo niza tamba mo tekanya kuona vamene azaniuza namwamene niza chokela kuma dandaulo yanga. ² Yehova ananiyanka naku kamba kuti, "Lemba menso mpenya aya, ulembe pamyala ilibe chili chonse kuti wamene wamene ayabelenga akazitamanga. ³ Pakuti menso mpenya yalindila ntawi yamusogolo ndipo yazakamba osakangiwa. Olo kuti yaka chedwa, mukayalindile. Chifukwa zoona yazakabwela ndipo siyaza dikila. ⁴ Ona! Wamene vofuna vake sivi vomelezana navili mukati mwake ni wozitukumula. Koma bolungama bazankalila pa chikulupililo chake. ⁵ Pakuti vinyu ima nama boza kuli munyamata ozitukumula kuti asakonkeke, koma akulise volaka laka vake monga manda na, monga infa, simakutila. Amazi sonkanisila eka ma ziiko yonse naku zisonkanisila eka bonse bantu. ⁶ Nanga ivi vonse siviza pangisa kukamba koomunyoza na nyimbo yobabisa mutima yokamba pali iye, kukamba kuti, soka kwa iye wamene apakisa vamene sivili vake! Uzasimikiza kwantawi itali bwanji kuonjezela volema vamene watenga?" ⁷ Nanga abo bamene bakuluma sibazanyamuka manje manje, nabamene baku yofya kuushiwa? Uzankala chovutisa kuli beve. ⁸ Chifukwa unafunka bantu bambili, bantu bosalako bonse baza kufunka. Pakuti una tila magari yabantu naku chita chiwawa pa malo, mumizinda, napali abo bamene bankalamo. ⁹ 'Soka kuli iye wamene asema nyumba yake kupitila mukapezedwe koipa, kuti aike nchisa yake pamwamba kuzipulumusa mu manja ya choipa.' ¹⁰ Waziletela nsoni munyumba yako paku juba bantu bambili, ndipo wachimwa pa iwe weka. ¹¹ Pakuti myala izalila mu vipupa, na mutanda wa mapulanga uzayazi yanka, ¹² 'Soka kuli iye wamene amanaga muzinda na magari, nawamene ankazikisa munzi musali muchilungamo.' ¹³ Nanga sichichokela kuli Yehova wamakamu kuti bantu basebenzela mulilo nama ziiko yonse yenangu yazivutisa pachabe? ¹⁴ Koma malo ya zula na chizibiso cha ulemelo wa Yehova monga manzi yavinikila pa nyanja. ¹⁵ 'Soka kuli iye wamene apatikiza banzake kumwa chakumwa_ ulangiza ukali wako footnot mopitilila naku bapangisa kuti bamwe ku oona vintako vao. ¹⁶ Uzazula na nsoni mumalo mwa ulemelelo. Manje nintawi yako! Imwa, ndipo uzalangiza kusadulidwa kwako! Chiko chamene chili ku zanja lamanja la Yehova chizabwela kuku zunguluka, na manyazi yazavinikila ulemelelo wako. ¹⁷ Chiwawa chamene chachitiwa kuli Lebanoni chizakuvutisa na chionongeko cha vinyama chizakuyofya. Pakuti watila magari yabantu naku chita chiwawa pa malo, mizinda, nabonse bamene bankalamo. ¹⁸ Nanga fano losema yaku chitila chani? Pakuti wamene anai sema, kapena wamene anapanga nsimbi nimupunzisi waboza; pakuti akulupilila nchito zamanja pamene apanga milungu zosakamba. ¹⁹ 'Soka kuli iye wamene akamba ku ma planga, ukani! Kapena kumyala zosakamba, Nyamukani! Nanga ivi vintu vima punzisa? Onani, nivopangiwa na golide na siliva, koma sivipema nangu pangono peka. ²⁰ Koma Yehova ali mu tempele yake yoyela! Nkalani zee pamenso pake, malo yonse."

Chapter 3

¹ Pempelo ya Habakuku muneneli: ² Yehova, nanvela mbili yanu, ndipo nayopa. Yehova, uukisani nchito yanu mukati mwa ntawi iyi; chipangeni chozibika mukati ka ntawi iyi. Kumbukilani kunkala na chifundo muku kalipa kwanu. ³ Mulungu anabwela kuchokela ku Temani, na oyela kuchokela ku Parani. Sela ulemelelo waka una vinikila kumwamba, na ziko lapansi inazula na chiyamiko. ^{4 5} Na kuwala kwake monga zuba, kuwala kuchokela mumanja mwake; mwamene umo anabisa mpavu zake. Matenda yamene yaleta infa yana enda pasogolo pake, na matenda yana mukonka. ⁶ Anaimilila nakupima ziko lapansi; analangana naku nyanganyisa ma ziiko. Ngakale ma pili yamu yayaya yana gumuka, na tuma pili twamu yayaya tuna gwada pansi. Njila yake sisila. ⁷ Ninaona ma hema yama Cushani muma vuto, na nyula zamu chihema kunjenjema muziko ya Midiani. ⁸ Nanga Yehova anali okalipa namimana? Nanga mukwiyo wanu unali pali mimana, kapena kukalipa kwanu pali nyanja, pamene munakwela pali makavalo yanu napali magaleta yanu yopambana? ⁹ Mwachosa uta wanu kopanda choivinikila; mwiaka mivi ku uta wanu! Ganizapo una gabanisa ma ziiko na mimana. ¹⁰ Mapili yanakuona naku pombana mu vobaba. Chigumula chamanzi chinapita; pansi panyanja pana punda. Ina nyamula mafunde. ¹¹ Zuba na mwezi vinaimilila mumalo mwake pakuwala kwa mivi zanu pamene zimbululuka, pakuunika kwa mukondo wako owala. ¹² Waenda enda paziiko lapansi namukwiyo. Mokalipa unadyaka dyaka maziiko. ¹³ Unaenda kunja chifukwa chachipulumuko cha bantu bako, pa chipulumuko chaozozedwa bako. Umwaza mukulu wanyumba yao ipa kunkala osavala kuchokela pansi kufikila kumukosi. Ganizapo ^{14 15} Walasa mutu wamukulu waba nkondo na mivi yake mwini pakuti babwela monga chimpepo chikulu kuti mwaza; kutamangila kwao kunali monga kwa iye wamene aononga bovuutika mumalo yobisika. Unaenda pamwamba pa nyanja naba kavalo bako, naku faka pamozi manzi yampanvu. ¹⁶ Ninanvela, na vamukati mwanga vina yopa! Milomo yanga ina njenjema pali chinanveka. Kuola kwabwela muma fupa yanga, ndipo pansi paina ninjenjemela pamene nilindila mwachete siku yachisoni kubwela pali bantu bamene banatingenela. ¹⁷ Nangu mutengo wa mukuyu supukila ndipo kulibe kubala kuchokela kuli mpesa; nangu kuti kubala kwa mutengo wa olivi kunakanga na minda sinabale vakudya vilivonse; nangu kuti vibeto vina jubiwa kuchokela mukola ndipo kulibe ng'ombe mukola, ichi ndiye chamene nizachita. ¹⁸ Koma, nizakondwela muli Yehova. Nizakondwela chifukwa cha Mulungu wa chipulumuso changa. ¹⁹ Ambuye Yehova nimpanvu yanga amapanga mapazi yanga monga mbawala. Amani pangisa kuyenda pasogolo mumalo yanga yapa mwamba. Kuli osogolela nyimbo, pa zingwe zosebenzesa

Zephaniah

Chapter 1

¹ Aya ndiye mau ya Yehova yamene yana bwela kuli Zefania mwana mwamuna wa Cushi mwana mwamuna wa Gedalia mwana mwamuna wa Amaria mwana mwamuna wa Hezekia, muma siku ya Josia mwana mwamuna wa Amosi, mfumu ya Yuda. ² "Nizaononga vonse vapa ziko lapansi_ ichi ndiye chizibiso cha Yehova. ³ Nizaononga muntu na navi nyama; Nizaononga nyoni zamu mwamba na nsomba zamumi mana, voonongeka pamozi navoipa. pakuti niza chosa muntu kuchokela paziko lapansi_ ichi ndiye chizibiso cha Yehova. ⁴ Niza tambasula kwanja yanga pali Juda napali bonse bonkala mu Jerusalemu. Nizajuba bonse bosala muli Baala kuchokela ku malo yake nama zina ya bantu mafano pakati paba nsembe, ⁵ bantu bamene bapembeza za kumwamba, nabantu bamene bapembeza naku lumbila kuli Yehova koma futi balumbila pali mfumu yao. ⁶ Niza juba futi na abo bamene baleka kukonka Yehova, abo bamene sibasakila Yehova kapena kufunsa malangizo yake." ⁷ Nkalani zee pamenso ya Yehova! Pakuti siku ya Yehova ilipa fupi; Yehova akonza nsembe naku faka pambali balendo bake. ⁸ "Chiza chitikapa pasiku ya nsembe ya Yehova, kuti niza langa mwana wamfumu mukazi na bana banfumu bamuna, nabonse balivale vovala vachilendo. ⁹ Pa siku iyo niza langa bonse abo bamene ba jumpa pamwamba pongenela, abo bamene bazuzya nyumba mbuya wao na chiwawa naboza. ¹⁰ Ndyi mwamene chizakankalila pasiku ija_ ichi ndiye chizibiso cha Yehova_ kuti kulila konzunzika kuzachokela pongenela poitanidwa Nsomba, kulila mokuwa kuchokela mu Dela yachibili, naku pwanyika konveka kukulu kuchokela mutu ma pili. ¹¹ Kuwani, bonkala muma Dela yamu ma maliketi, pakuti ba malonda bonse baza onongeka; bonse bamene bapima siliva baza jubiwa. ¹² Chizafika pantawi ija pamene niza sakila sakila Jerusalemu nama lampi naku langa bazimuna bamene bankalila mu vinyu vao nakukamba mumitima zao, 'Yehova sazachita chili chonse, chabwino kapane choipa.' ¹³ Chuma chao chizatengewa, na manyumba yao yazankala yoonongeka yalibe bonkalamo! Baza manga

manyumba koma sibaza nkalamo, naku shanga minda yampesa koma osamwako vinyu wake.¹⁴ Koma ine, ili ndi pangano langa ndi iwo, ati Yehova, mzimu wanga uli pa iwe, ndi mawu anga amene ndaika mkamwa mwako, sadzachoka pakamwa pako, kapena kupita. Tsiku lalikulu la Yehova layandikira, lili pafupi. kufulumira!¹⁵ Phokoso la tsiku la Yehova lidzakhala la wankhondo amene adzalira kwambiri! Tsiku limenelo lidzakhala tsiku la mkwiyo, tsiku losautsa ndi losautsa, tsiku la namondwe ndi chiwonongeko, tsiku lamdima ndi lachisoni, tsiku lamitambo ndi lamdima wandiweyani.¹⁶ Lidzakhala tsiku la malipenga ndi maphokoso pa mizinda yokhala ndi mipanda yolimba kwambiri.¹⁷ Pakuti ndidzadzetsa masautso pa anthu, kuti adzayendayenda ngati anthu akhungu popeza adachimwira Yehova. Magazi awo adzatsanulidwa ngati fumbi, ndi mkati mwawo ngati ndowe.¹⁸ Siliva kapena golide wawo sadzakhoza kuwapulumutsa pa tsiku la mkwiyo wa Yehova. Ndi moto wa nsanje yake dziko lonse lapansi lidzawotchedwa, pakuti iye adzawonongeratu anthu onse okhala padziko lapansi.

Chapter 2

¹ Sonkhanitsani ndi kusunkhana, inu anthu osachita manyazi - ² lamulolo lisanayambe kugwira ntchito ndipo tsikulo likadutsa ngati mankhusu, mkwiyo woyaka wa mkwiyo wa Yehova usanakugwereni, lisanakugwereni tsiku la mkwiyo wa Yehova. ³ Funani Yehova, inu nonse odzichepetsa padziko lapansi amene mumvera malamulo ake! Funafunani chilungamo. Sakani kudzichepetsa, ndipo mwina mudzatetezedwa tsiku la mkwiyo wa Yahweh ⁴ Pakuti Gaza adzasiyidwa; ndi Asikeloni adzasanduka bwinja. Adzapitikitsa Asidodi masana, ndipo adzazula Ekroni! ⁵ Tsoka kwa okhala m'mbali mwa nyanja, mtundu wa Akereti! Yehova wanena za iwe, Kanani, iwe dziko la Afilisiti. Ndidzakuwononga kufikira kuti sipadzakhala wokhalamo. ⁶ Motero gombe lidzakhala busa la abusa ndi makola a nkhusa. ⁷ Dera lakugombe lidzakhala la otsala a nyumba ya Yuda, amene adzaweta nkhusa zawo kumeneko. Anthu awo adzagona madzulo m'nyumba za Asikeloni, pakuti Yehova Mulungu wawo adzawasamalira, nadzabwezeretsa chuma chawo. ⁸ "Ndamva kutonza kwa Mowabu ndi kunyoza kwa ana a Amoni pamene anatonza anthu anga ndi kuwononga malire awo. ⁹ Chifukwa chake, pali Ine, ati Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, Moabu adzakhala ngati Sodomu ndipo anthu a Amoni ali ngati Gomora; malo a lunguzi ndi dzenje lamchere, lopanda kanthu kosatha. Koma anthu anga otsala adzawalanda, ndi otsala a mtundu wanga adzawatenga. " ¹⁰ Izi zichitikira Moabu ndi Amoni chifukwa cha kunyada kwawo, popeza adanyoza ndi kunyoza anthu a Yehova wa makamu. ¹¹ Pamenepo adzaopa Yehova, pakuti adzatonza milungu yonse ya padziko lapansi. Aliyense adzambulambira, aliyense kuchokera kwawo, kuchokera kunyanja iliyonse. ¹² Akusiya nawonso adzaphedwa ndi lupanga langa, ¹³ ndipo dzanja la Mulungu lidzaukira kumpoto ndi kuwononga Asuri, kotero kuti Nineve adzakhala bwinja lopanda bwinja ngati chipululu. ¹⁴ Ndipo ng'ombe zidzagona pansi pomwepo, nyama zonse za amitundu; zonse kadzidzi ndi kadzidzi zikukhala pamwamba pazipilala zake. Kuitana kudzayimba m'mazenera; zinyalala zidzakhala pakhomo. matabwa ake a mkungudza adzaonekera poyera. ¹⁵ Uwu ndi mzinda wokondwa womwe unkakhala wopanda mantha, womwe mumtima mwake umati, "Ndine, ndipo palibe wofanana ndi ine." Iye wakhala chinthu chodabwitsa, malo ogona nyama. Aliyense amene amadutsa pafupi ndi iye adzaimbira mluzu ndi kumugwetsera nkhuja.

Chapter 3

¹ Tsoka mzinda wopandukawo! Mzinda wachiwawa waipitsidwa. ² Sanamvere mawu a Mulungu, kapena kulandira chilango kuchokera kwa Yahweh. Sakhulupirira Yehova ndipo sadzafikira Mulungu wake. ³ Akalonga ake ali ngati mikango yobangula pakati pake. Oweruza ake ndi mimbulu yamadzulo yomwe siyisiya kalikonse kuti idyedwe m'mawa. ⁴ Aneneri ake ndi anthu achipongwe ndi achiwembu. Ansembe ake aipitsa choyera napotoza chilamulo. ⁵ Yehova ali wolungama pakati pake; Iye sangachite cholakwika chilichonse. M'mawa ndi m'mawa adzapereka chiweruzo; Sichidzakhala kobisika poyera, koma anthu osalungama sachita manyazi. ⁶ "Ndawononga mitundu ya anthu; nyumba zawo zowonongedwa zawnongedwa. Ndasandutsa makwalala awo kuti pasapezeke wina wowadutsa. Mizinda yawo yawonongedwa ndipo palibe munthu amene akukhalamo. ⁷ Ndinati, 'Zoonadi mudzandiopa. Landirani Konzani ndipo musadulidwe m'nyumba zanu ndi zonse ndalingalira kukuchitirani. Koma anali ofunitsitsa kuyamba m'mawa uliwonse ndikuwononga zochita zawo zonse. ⁸ Chifukwa chake dikirani ine, ati Yehova, kufikira tsiku ndidzayimilira kulanda nyama. Pakuti ndaganiza zosonkhanitsa amitundu, kusonkhanitsa maufumu, kutsanulira pa iwo mkwiyo wanga, mkwiyo wanga wonse woyaka moto; pakuti ndi moto wa nsanje yanga dziko lonse lapansi lidzawonongedwa. ⁹ Koma pamenepo ndidzayeretsa milomo ya anthu, kuti iwo onse atchule dzina la Yehova kumtumikira ndi mtima umodzi. ¹⁰ Opembedza anga, anthu anga akubalalika, abwera tsidya lija la mtsinje wa Kusi, adzabwera ndi zopereka kwa ine. Tsiku lomwelo simudzachita manyazi chifukwa cha zonse munandichitira ine, ¹¹ popeza nthawi yomweyo ndidzachotsa pakati panu amene anakondwera ndi kudzikiza kwanu, ndi chifukwa chakuti simudzachitanso kanthu modzikiza paphiri langa loyera. ¹² Koma ndidzasiya pakati pako anthu aumphawi ndi aumphawi, ndipo adzapeza pobisalira m'dzina la Yehova. ¹³ Otsalira a Israyeli sadzapanganso zopanda chilungamo kapena kunena zonama, ndipo palibe lilime lachinyengo lomwe lidzapezeke pakamwa pawo; ndipo zidzadya ndi kugona pansi, ndipo palibe wakuwawopsa." ¹⁴ Imba, iwe mwana wamkazi wa Ziyoni; Fuula, Israeli. Kondwera ndi kusangalala ndi mtima wako wonse, iwe mwana wamkazi wa Yerusalemu. ¹⁵ Yehova wachotsa chilango chako; wathamangitsa adani ako! Yehova ndi mfumu ya Israeli pakati panu. Simudzaopanso choipa! ¹⁶ Tsiku lomwelo adzati kwa Yerusalemu, Usaope Ziyoni, manja ako asafowoke; ¹⁷ Yehova Mulungu wako ali pakati pako, wamphamvu kuti akupulumutse. Iye adzakondwerera chifukwa cha iwe ndi chimwemwe; adzakhala chete pa inu mchikondi chake; adzakondwera nawe, nadzakondwera. ¹⁸ Ndidzasonkhanitsa iwo omwe akumva chisoni, omwe sangathe kupita kumaphwando osankhidwa, kuti musakhalenso ndi manyazi chifukwa cha izi. ¹⁹ Taonani, nditsala pang'ono kutsutsana ndi adani anu onse. Pa nthawi imeneyo, ndidzapulumutsa olumala ndi kusonkhanitsa pamodzi anthu otayika. Ndipo ndidzawasandutsa ayamikidwe, ndi kusanduliza manyazi awo akhale mbiri ya dziko lonse lapansi. ²⁰ Nthawi imeneyo ndidzakutsogolera; nthawi imeneyo ndidzakusonkhanitsa. Ndidzachititsa kuti mitundu yonse ya padziko lapansi ikuopeni ndi kukutamandani, mukaona kuti ndakubwezeretsani, "watero Yehova.

Haggai

Chapter 1

¹ Mu chaka cha chibili cholamulila cha Daliyasi mfumu, mu mwezi wa nambala sikisi, pa siku yoyamba ya mwezi, mwau ya Yehova yanabwela kupitila mu kwanja ya Hagai muneneli kuli Kazembe wa Yuda, Zelubabelo mwana wa Shiyatelo, nakuli mukulu wansembe Yohuwa mwana wa Jezodaki, kukamba kuti, ² "Yehova wa makamo aka kuti: Aba bantu bakamba kuti, 'Sintawi yamene ise tiyenela kubwela kapena kumanga nyumba ya Yehova.'" ³ Pamene apo mau ya Yehova yanabwela kupitila mumanja ya Hagai muneneli, kukamba kuti, ⁴ "Nanga iyi ni ntawi yakuti imwe mweka mukazinkala mumanyumba yanu yomangiwa bwino, koma iyi nyumba inkala yo-onongeka?" ⁵ Manje apa Yehova wamakamo akamba kuti: Ganizani poni pali njila zanu! ⁶ Mwashanga mbweu zambili, koma mukolola vokolola ving'ono; mukudya koma simukuta; mukumwa koma simukolewa. Muvala vovala koma simutuma, nauja wanchito wamene amafola ndalama amaika mutumba yamene niyotulika! ⁷ Yehova wamakamo akamba kuti: "Ganizani poni pali njila zanu! ⁸ Endani kuma pili, katengeni mitengo, mumange nyumba yanga; ine nizamvela bwino kwambili, ndipo nizapasiwa ulemelelo!-akamba Yehova." ⁹ "Munasakila vambili, koma onani! mwaleta vochepe kunyumba, chifukwa inwe ninafunzililapo! Nanga?" akamba Yehova wamakamo. "Chifukwa nyumba yanga nio-onongeka, koma muntu ali onse akonza

nyumba yake. ¹⁰ Chifukwa cha ichi makumbi yanagwililila mvula yanu, na ziko inagwila vokolola vanu. ¹¹ Naitana chilala pa ziko na pama pili, pa mbeu na pa vinyu va manje, pa mafuta na pa vokolola vapa ziko, pa bantu na pa vinyama, na pa zinchito zonse za manja yanu!" ¹² Pamene apo Zelubabo mwana wa Shiyatiyelo, na mukulu wansembe Yoshuwa mwana wa Jehozadaki, pamozi na bosalapo pa bantu, bana mvela mau ya Yehova Mulungu wabo na mau ya Hagayi muneneli, chifukwa Yehova Mulungu wabo anamutuma na bantu bonse banayopa nkope ya Yehova. ¹³ Pamene apo Hagayi, mutumiki wa Yehova, anapeleka utenga wa Yehova ku bantu nakukamba kuti, "Nili naimwe!-ichi ndiye chamene Yehova akamba!" ¹⁴ Yehova anazizimula muzimu wa kazembe wa Yuda, Zelubabo mwana wa Shiyatiyele, na muzimu wa mukulu wa nsembe Yoshuwa mwana wa Jehozadaki, na muzimu wa bonse bosalapo ku bantu, mwakuti bana enda naku sebenza mu nyumba ya Yehova wamakamo, Mulungu wabo ¹⁵ pa siku ya 24 mu mwezi wa namba six, chaka cha chibili cha Daliyasi mfumu.

Chapter 2

¹ Mu mwezi wa namba seven pa siku ya namba 21 ya mwezi uja, mau ya Yehova yanabwela kupitila mumanja ya Hagayi muneneli, kukamba kuti, ² "Kamba na Kazembe wa aYuda, Zelubabo mwana wa Shiyateyelo, na kuli mukulu wansembe Yohuwa mwana wa Yehozadaki, nakuli bosalapo ku bantu. Ukambe kuti, ³ 'Kansi nindani wamene anasalapo pakati panu wamene anaona iyi nyumba mu ulemelelo wake wakudala? Nanga manje muiona bwanji? Kansi si ioneka yachabe mumenso yanu? ⁴ Manje, limba, Zelubabewo!-uku ndiye kukamba kwa Yehova-naiwe unkale olimba, mukulu wansembe Yeshuwa mwana wa Jehozadaki; munkale bolimba, bonse bantu bamu ziko!-uku ndiye kukamba kwa Yehova-sebenzani, chifukwa ine nili na imwe!-uku ndiye kukamba kwa Yehova wamakamo. ⁵ Iyi ndiye pangano yamene ine ninankazikika pamene munachoka ku Igupto, na Muzimu wanga ukali naimwe. Musayope! ⁶ Chifukwa Yehova wamakamo akamba ichi: Kwa kantawi kangono nizagwedeza mwamba na pansi, njanja na ntaka palibe manzi! ⁷ Nizagwedeza ziku ili yonse, ndipo ziko ili yonse izaleta vintu vamutengo wapatili kuli ine, ndipo nizazulisa nyumba yanga na ulemelelo, akamba Yehova wamakamo. ⁸ Siliva na golide niyanga!-uku ndiye kukamba kwa Yehova wamakamo. ⁹ Ulemelelo wa nyumba iyi uzankala ukulu kusogolo kuchila poyambila, akamba Yehova wamakamo, ndipo nizapeleka mutendere mumalo aya!-uku ndiye kukamba kwa Yehova wamakamo." ¹⁰ Pa siku ya 24 ya mwezi wa nine, mu chaka chachibili cha Daliyasi, mau ya Yehova yanabwela kupitila muli Hagayi muneneli, kukamba kuti, ¹¹ "Yehova wamakamo akamba kuti, Bafunseni bansembe pali lamulo, mukambe kuti, ¹² 'Ngati mwamuna anyamula nyama yamene inapatuliwila Yehova mutumba ya chovala chake, ndipo ntumba ija yakumya buledi kapena supu, vinyu kapena mafuta, kapena chakudya chilichonse, nanga izankala yoyela?" Wansembe anayanka kukamba kuti, "Iyayi." ¹³ Pamene apo Hagayi anakamba kuti, "Ngati ali onse wamene ali na doti chifukwa cha imfa agwila chili chonse pali ivi, nanga ama nkala osapatulika?" Bansembe banayanka nakukamba kuti, "Zo-ona, bankala nadoti." ¹⁴ Pamene apo Hagayi anayanka naku kamba kuti, "Nichimozi-mozi na bantu aba na ziko iyi pa menso panga!-uku ndiye kukamba kwa Yehova-ndiye mwamene chilili mu nchito zabo za manja yabo. Vonse vamene bapele nivadoti! ¹⁵ Manje apa, ganizani pa ntawi za kumbuyo uku mpaka kufika siku ya lelo. Pamene mwala ulionse usanaikiwe pa mwala wina mu tempele ya Yehova, ¹⁶ nanga inali bwanji paja? Pamene munakwanisa ma unjika yokwanila twenty ya mbeu, yanali kukwanila chabe ten; na pamene muna bwela konzungila vinyu kuti mutapemo migomo zili 50, zinakwanamo chabe 20. ¹⁷ Ninakuvutisani mu nchito za manja yanu kupitila mu kusungulumwa na nkungu, koma imwe simunatembenukile kuli ine-uku ndiye kukamba kwa Yehova. ¹⁸ Ganizanipo kuyambila siku yalelo kuyenda kusogolo, kuyambila siku ya 24 ya mwezi wa nine, kuchokela siku yamene maziko ya nyumba ya Yehova yana nkazikisika. Ganizaniponi! ¹⁹ Nanga ikalimo mbeu mu nkokwe? Vinyu, mutengo wa mukuyu, mankhusu, na mitengo zama olivu sizina bale! Koma kuyambila siku yalelo nizakudalisani imwe!" ²⁰ Manje mau ya Yehova yanabwela kachibili kuli Hagayi pa siku ya 24 ya mwezi kukamba kuti, ²¹ "Uza kazembe wa aYuda, Zelubabelo, ukambe kuti, 'Nizagwedeza mwamba na pansi. ²² Chifukwa ine nizagwesa mipando za mafumu naku ononga mpavu zama ufumu za maiko! Nizagwesa ma galeta na boya enza; ma kavalo na boyakwela bazagwa pansi, ali onse chifukwa cha lupanga wa mubale wake. ²³ Pa siku ija-uku ndiye kukamba kwa Yehova wamakamo-Nizakutenga iwe, Zelubabo mwana wa Shiyatiyelo, monga wanchito wanga-uku ndiye kukamba kwa Yehova. Nizakulenga kunkala mpete yodindila, chifukwa ine nakusanka! -uku ndiye kukamba kwa Yehova wa makamo!"

Zechariah

Chapter 1

^{1 2 3} 1 mumwezi wa 8 muchaka cha chibili cha ulamulilo, wa darius, mau ya YEHOVA yanabwela kuli zekariya mwana mwamuna wa berekiya mwana mwamuna wa ido, muneneli, kukamba, 2"YEHOVA ana kwiya maningi na mazi tate yanu! 3kamba kuli beve, YEHOVA wamakamu akamba ichi: bwelani kuli ine!-uku nikukamba kwa YEHOVA wa makamu- ndiponso nizabwelela kuli imwe, akamba YEHOVA wa makamu. ^{4 5 6} 4 musankale monga ba zitate banu bamene ba neneli bana lilila kumbuyo uku, kukamba, "YEHOVA wa makamu akamba ichi: chokani kuma yendedwe yanu ya uchimo na vochita vanu voyipa!" koma sibana fune kuvela ndiponso sibana ike nzelu kuli ine-ivi nivokamba va YEHOVA, 5 mazitate yanu, yali kuti? ba neneli bali kuti, nanga bali pano muyayaya? 6koma mau yanga na vokamba vanga vamene nina lamulila ba kapolo banga ba neneli, sivina yende

pa sogolo pa mazi tate yanu? mwa ichi bana tembenuka na kukamba, 'monga mwamene YEHOVA wa makamun enzo ganizila kuchita kuli ise vamene mayendedwe na ma chitidwe yatu yenzo yenela, ndipo atichita vamene ivo, ""^{7 8 9} 7pasiku ya 24 mumwezi wa 11, wamene uli mwezi wa sehati, muchaka cha chibili mu ulamulilo, wa dariusi' mau ya YEHOVA yana bwela kuli zekariya mwana mwamuna wa berekiya mwamuna wa ido, muneneli, kukamba, 8"nina wona usiku, na , kuyangana! mwamuna ninshi akwela pa kavalo yo fira, ndipo anali mukati mwa mitengo za masamba zili mu chigwa; ndipo kumbuyo kwake kunali aka valo bo fira, bo sweta na boyera." 9nina kamba, "nivichani ivi vintu, ambuye?" ndipo mungeli enzo kamba na ine ana kamba kuli ine, "nizakulangiza kuti ivi vintu nivi chani."^{10 11} 10ndipo mwamuna enze ana yimilila pakati pa mitengo za masamba ana yanka, "aba ni abo YEHOVA atuma kuyenda muziko yonse ya pansi kuyenda yenda." 11 bana muyanka mungeli wa MULUNGU wamene ana yimilila pakati pa mitengo za masamba; bana kamba kuli eve, "tanka tingo yenda yenda mu ziko yonse ya pansi; ona, ziko yonse inkala ili zii ndiponso ili pa mupumulo."^{12 13} 12ndiponso mungeli wa YEHOVA una yanka na kukamba, "YEHOVA wa makamu, muzankala ntawi itali bwanji kulibe kulangiza chifundo kuli yelusalema na ku mizinda za yuda, yamene mwankala muli nayo na ukali pa zaka 70?" 13 YEHOVA ana yanka mungeli wamene enze ana kamba na ine, na mau yabwino, mau yo tontoza.^{14 15} 14ndipo mungele enze ana kamba na ine anakamba kuli ine, "itana na kukamba, 'YEHOVA wa makamu akamba ivi: nankala ni chitila nsanje yelusalema ndiponso ziyoni na chilako lako chikulu! 15ndine okalipa maningi na mayiko yali pa mutendele. pamene nenze wokalisa che pa ng'ono na beve, ba vionongelatu vintu."^{16 17} 16 mwa ichi YEHOVA wa makamu akamba ichi: nabwelela kuli yelusalema na chifundo chambili. nyumba yanga iza mangiwa mukati mwake- aya ndiye mau ya YEHOVA wa makamu-ndiponso ntambo yo pimila iza tambasuliwa kunja kuli yelusalema! 17 futi uyitane, kukamba, 'YEHOVA wamakamu akamba ivi: mizinda yanga iza taikila futi na vabwino, ndiponso YEHOVA aza tontoza futi ziyoni, ndiponso aza sanku futi yelusalema.'"^{18 19} 18 ndiponso nina nyamula menso yanga kumwamba na kuona nsengo zili 4! 19nina kamba na mungeli anakamba na ine, "nivichani ivi?" ana niyanka. "izi ni nsengo zamene za palanganya yuda, isilayeli, na yelusalema." 20 ndipo YEHOVA ananilangiza bobbeza bali 4. 21nina kamba, "aba bantu ba bwela kuchita chani?" anayanka, na kukamba, "izi ni nsengo zina palanganya yuda kuti kusankale muntu lai wonse wonyamula muttu. koma ba misiri babwela kuba yofya. kugwesa nsengo za mayiko yamene yana nyamula nsengo yao kuyofya ziko

Chapter 2

^{1 2} 1chokonkapo nina nyamula menso yanga kumwamba nakuona muntu na ntambo yopimilako mumanja mwake. 2ninakamba, " uyenda kuti?" ndipo anakamba kuli ine, "kupima yelusalema, kuona ukulu na utali wake." ^{3 4 5} ndipo mungeli wamene tina kambisana naye ana chokapo ndiponso mungeli winango anachoka panja kuyendo kumana na eve. 4mungeli wa chibili anakamba kuli eve, " tamanga ndiponso ukambe kuli munyamata uja; kuti, 'yelusalema azankala ziko yoseguka chifukwa chakupaka kwa bantu na vibeto mukati mwake. 5pakuti ine-uku nikukamba kwa YEHOVA-nizankala kuli eve chipupa cha mulilo cho muchingiliza, ndiponso nizankala ulemelelo pakati pake. ^{6 7} 6 nyamuka! nyamuka! tabamo muziko ya kumpoto- uku nikukamba kwa YEHOVA-pakuti na kupalanganyani monga mpepo zili 4 za mumlengalenga!- uku nikukamba kwa YEHOVA. 7nyamuka! tabila ku ziyoni, iwe wamene unkala na"" mwana mukazi wa babiloni! ^{8 9} YEHOVA wa makamu anani lemekeza ine na kunituma kuma yiko yamene yana ku vutisa-mwa ichi ali wonse wogwila iwe, agwila ka pakati pa linso ya MULUNGU!-pambuyo pochita ivi YEHOVA, anakamba, 9"ine neka niza nyamula kwanja yanga pali beve, bakapolo bao bazabapoka katundu yao." mwa ichi uzaziba kuti YEHOVA wa makamu anituma. ^{10 11} 10imbila chisangalalo, mwana mukazi wa ziyoni, pakuti ine mwine wake nibwela kunkala pakati panu!-uku nikukamba kwa YEHOVA." 11ndiponso mayiko yakulu yaza zilumikizakuli YEHOVA musiku ija. akamba, "ndiponso muzankala bantu banga; pakuti nizankala pakati panu," ndipo muzaziba kuti YEHOVA wa makamu anituma kuli imwe. ^{12 13} 12pakuti YEHOVA aza tenga yuda ngati choloba ngati katundu yake yoyenela mu malo yoyela ndiponso azazisankila futi yelusalema. 13nkala zee, wa tupi onse, pamenso pa YEHOVA, pakuti anyamuliwa kuchoka ku malo yake yoyela!

Chapter 3

^{1 2 3} 1ndiponso YEHOVA ananilangiza yoswa mukulu wansembe ayimilila pamenso pa mungeli wa YEHOVA na satana anali imilile ku kwanja yake ya manja kumupasa muladu wa uchimo. 2mjungelo YEHOVA anakamba kuli satana, "YEHOVA akuzuzule, satana; YEHOVA, wamene asanka yelusalema, akuzuzule! kodi sichi nkuni chachosewa mu mulilo?" 3yoswa enze ovala vovala va doti pamene ana imilila pa menso pa mungeli. ^{4 5} mungeli anakamba anati kuli abo benze imilile pamenso pake, "muchoseni vovala va doti. " ndipo anakamba kuli yoswa, "yangana! nale 5ngesa machimo yako ku choka pali iwe ndipo niza kuvalika vovala vabwino." ndipo nina kamba, "mu ikeni chisote chosaifpa pa mutu pake!" ndipo bana ika chisote chosafipa pa mutu wa yoswa na kumuvalika vovala vilibe doti, pamene mungeli wa YEHOVA anali imilile. ^{6 7} 6chokonkapo mungeli wa YEHOVA analamulila yoswa na kukamba, 7"YEHOVA wa makamu akamba ichi: ngati uzayenda munjila zanga, ndiponso ngati uza sunga malamulo yanga, ndipo uza lamulila nyumba yanga na kulonda malo yanga yakunja, pakuti nizakuvomeleza kuyenda na kubwela pakati pa aba bamene ba imilila pa menso panga. ^{8 9} mvela, yoswa mukulu wansembe, iwe na banzako bamene bankala na iwe! pakuti aba bantu ni cho onelako, pakuti ine neka niza nyamula kapolo wangaali ni ntambi. 9 manje ona mwala wamene na ika pamenso pa yoswa. pali menso yali 7 pa mwala umozi uyu, ndipo nizalembapo mau-uku ni kukamba kwaYEHOVA wa makamu- ndiponso niza chosa uchimo mu malo aya musiku imozi. ¹⁰ musiku ija-uku ni kukamba kwa YEHOVA wa makamu-ali onse muntu azaitana munzake kunkala pansu pa mutengo wake wa mpesa na pansu pa mutengo wake wa mkuyu."

Chapter 4

^{1 2 3} 1ndipo mengeli enzo kambisana na ine ana chunguluka na kuni nyamula monga muntu wamene anyamuliwa mu tulo. 2anakamba kuli ine, "uona chani?" nina kamba, "niona choikapo nyali chopangiwa na golide yeka, na mbale pamwamba pake. chili na nyale zili 7 ndiponso-----pamwamba pa nyali ili yonse. 3 mitengo zibili za mpesa zili pa mbali, umozi ku mbali ya kwanja ya manja ya mbale ndiponso inango ku mazhele." ^{4 5} 1mwa ichi ninakamba futi na mungeli wamene enze kukamba na ine. ninakamba, "ivi vintu vitantauza chani, mbuye wanga?" 5mungeli wamene enzo kamba na ine ana yanka na kukamba kuli ine, "siuziba kuti ivi vintu vitantauza chani?" nina kamba, "iyayi, mbuye wanga." ^{6 7} 6 ndipo anakamba kuli ine, "aya nimau ya YEHOVA kuli zerubabele: osati na mpamvu kapena kulimba, koma koma na muzimu wanga, akamba YEHOVA wamakamu. 7ndiwe chani, pili ikulu? pamenso pa zerubabele uzankala malo yalibe chintu, ndiponso azachosa mwala wa pamwamba ku punda kwa, chisomo! chisomo pali weve!" ^{8 9 10 11} 8mau ya YEHOVA bwela kuli ine, kukamba. 9"manja ya zerubabele yana ika maziko ya nyumba iyi ndiponso manja yake yaza isilizisa," mwa ichi muzaziba kuti YEHOVA wamakamu anituma kuli imwe. 10nindani anasula siku ya vintu ving'ono? aba bantu baza sangalala ndiponso kuona mwala wo ononga mukwanja ya zerubabele.(izi nyali zili 7 ni menso ya YEHOVA yamene ya yenda yenda pa ziko lonse lapansi. 11ndipo nina mufunsa mungeli, "nanga izi mitengo zibili za olivi zili kumazhele na kukwanja ya manja ya choikapo nyali?" ^{12 13} 12 futi ninamufunsa, "nanga izi ntambi zibili za olivi kumbali kwa mipopi zibili zagolide zamene zili na chotililako mafuta kuchoka mukati mwake?" ndipo anakamba kuli ine, "siu ziba kuti ivi ni vichani?" ninakamba, "iyayi, mfumu yanga." ¹⁴ 14ndipo anakamba, "aba ni bana bamuna ba olivi ya fresh bamene ba imilila pamenso pa AMBUYE ba ziko yonse."

Chapter 5

^{1 2} 1ndipo nina pindamuka na kunyamula menso yanga, ndipo ni naona, cholembelapo chimbululuka! 2mungelo anakamba na ine, "uona chani?" ninayanka, "niona cholembelapo chimbululuka, mupimo okwanila 20 mu utali ndiponso 10 mu ukulu." ^{3 4} ndipo anakamba kuli ine, "iyi nitembelelo yamene iyenda pa ziko yonse ya pansi. pakuti kawalala ali wonse az jubiwako kulingana na vamene vina lembewa kumbali inango, ndiponso ali wonse wamene alumbila va boza aza chosewako kulingana na vamene vina lembewa kumbali inango. 4"niza itumiza-uku nikukamba kwa YEHOVA wamakamu-mwa ichi izangena munyumba ya kawalala na munyumba ya wamene alumbila va boza pa zina yanga. izankalilila munyumba mwake na kuononga mitengo ya timba na myala." ^{5 6 7} ndipo mungeli wamene enzo kamba na ine anachoka panja na kukamba kuli ine, "nyamula menso yako na kuona chamene chibwela!" 6ninakamba, "nichani?" anakamba, "iyi ni swanda yamene ili nagondolo yamene ibwela. uyu ni uchimo wao muziko lonse." 7ndiponso chivininkilo china chosewapo pa swanda ndiponso munali muzimai pansi pake enze nkezi mukati mwa swanda! ^{8 9} 8mungeli anakamba, "uku nikuipisa!" anamuponya kumubweza mu swanda, ndiponso anabwezelapa chivalilo. 9 ninanyamula menso yanga nakuona bazimai ba bili babwela kuli ine, ndiponso pembo inali mumapapiko yao-pakuti banali na mapapiko monga ya kakowa. bana nyamula swanda pakati pa ziko na kumwamba. ^{10 11} ndipo nina kamba kuli mungeli wamene enzo kamba na ine, "bapeleka kuti swanda?" 11anakamba kuli ine, "ku imangila tempele mu ziko ya shinara, kuti tempele ikasila, swanda iza ikiwa pa malo yake yokonzewa."

Chapter 6

^{1 2 3 4} ndipo nina pindamuka na kunyamula menso yanga na kuona magaleta yali 4 yachokela pakati pa mapili ya bili; ndipo mapili yabili yopangiwa na bulonzi. 2galeta yoyamba yenze na akavalo bo fiira, galeta ya chibili inali na akavalo bo fipa, 3galeta ya chitatu inali na akavalo bo yela, ndiponso galeta ya chinai inali na akavalo ba mabala mabala. 4ndipo nina yanka na kukamba kuti kuli mungeli anakamba na ine, "nivichani ivi, mfumu yanga?" ^{5 6} mungeli anayanka na kukamba kuli ine, "izi nimpepo zili 4 zamumyamba zamene ziyenda panja kuchoka pamalo yamene zenzo yimililapa menso pa AMBUYE wa ziko yonse ya pansi. 6yamene ili na makavalo yo fipa ichoka iyenda ku ziko ya kumpoto; ma kavalo yo yela ya choka ya yenda kuziko ya kuvuma; na ba kavalo ba mabala mabala bayenda ku ziko ya kuvuma." ^{7 8} 7aya ma kavalo ya mpamvu yanachoka kufuna che kuyendo yenda yenda pa ziko yonse yapansi, ndipo mungeli ana kamba, "endani muka yende yende pa ziko ya pansi!" ndipo bana yenda pa ziko yonse yapansi. 8ndipo anani itana nakunikambisa kukamba kuti, "yangana abo bamene bayenda kuziko ya kumpoto; baza kondwelesa muzimu wanga pali ziko ya kumpoto." ^{9 10 11} 9mwa ichi mau ya YEHOVA yanabwela kuti ine kukamba, 10"tenga chopeleka kuchokela kuli bantu ba ku heledai, tobila, nayedaya-ndipo uyende lelo yamene na kuchipeleka munyumba ya yosiya mwana mwamuna wa zefaniya, wamene achoka ku babiloni. 11ndipo utenge siliva na golide, upange chisoti chaufumu na kuchiyika pa mutu pa yoswa mwana mwamuna wa yehozadaki, mukuluy wansenbe. ^{12 13} 12kamba naye, 'YEHOVA wa makamu akamba ichi: uyu muntu, zina yake ni buranchi! azakula kwamene alili ndiponso azamanga tempele ya YEHOVA, ndipo azavaliwa vovala va ufumu va bwino maningi, ndiponso azankala na kulamulila pamupando wake wa ufumu. azankala wansembe pa mupando wake wa ufumu. aznkala wansembe pa mupando wake wa ufumu, ndiponso azanyamula upungu wa mtendele pakati pa babili. ^{14 15} 14chisote cha ufumu chizapasiwa kuli heledai, tpbiya, yedaya, na heni mwan mwamuna wa zefaniya ngati chokumbukilako mu tempele ya YEHOVA. 15ndipo abo bamene bali kutali tali baza bwela kumanga tempele ya YEHOVA, mwa ichi uzaziba kuti YEHOVA wa makamu anituma kuli iwe; ivi viza chitika chabe ingati zoonza mwanvela ku liwu ya YEHOVA MULUNGU wanu!"

Chapter 7

^{1 2 3} 1pamene mfumu dariusi anankala pa zaka 4, pa siku ya 4 ya kislevi (wamene wenze mwezi wa 9), mau ya YEHOVA yana bwela kuli zekariya. 2bantu ba betele benze bana tuma sarezere na regemumereki na bantu bao kupempa pa menso pa YEHOVA. 3bana kamba na bansembe benzeli pa nyumba ya YEHOVA wa makamu na ba neneli; bana kamba, "nilile mu mwezi wa 5 na kusala kudya, monga mwamene nachitila zaka zambili izi?" ^{4 5 6 7} ndipo mau ya YEHOVA wa makamu yana bwela kuli ine kukamba, 5" kamba na bantu bonse ba paziko na kuba nsembe na kukamba, 'pamene muna sala kudya na kulila mu mwezi wa 5 na mumwezi wa 7 wa zaka izi zili 70, mwati munali kusalila ine kudya? 6pamene munamwa na kudya, simunazidyele na kuzimwela mweka? 7aya sindiye mau ya mozi na ya mozi yamene YEHOVA anakamba na kwanja ya ba neneli ba kudala, pamene yelusalema na mizinda yo muzunguluka ina nkaliwamo na kulemela, na ma negeva na mayiko yapansi kuyenda kumwera yana nkaliwamo?" ^{8 9 10} 8mau ya YEHOVA yanabwela kuli zekaraya, kukamba, 9"YEHOVA wa makamu akamba ichi, 'weluzani na chilungamo, ku kulupilika kwa pangano, na chifundo. lekani ali wonse muntu achite ivi kuchitila mubale wake. 10 apli wofedwa na wa masiye, na bakunja, na muntu wosauka-musabatitikize, ndiponso pakati panu pa sankale wo ganizila kuchita munzake voipa mumutima mwake.' ^{11 12} koma banakana kumvelela na kuchitisa ntota ma pewa yao. bana lekesa matu yao kuti yasamvele. 12banapanga mitima yao kulimba monga myala kuti basamvele lamulo ya mau ya YEHOVA wa makamu. anatumiza mau aya kubantu na muzimu wake muntau ya pachiyambi, na milomo ya baneneli. koma bantu banakana kumvela, ndipo YEHOVA wa makamu nakalipa nao. ^{13 14} pamene ana baitana, sibana nvele. mjunjila imozi," akamba YEHOVA wamakamu, "baza niyitana, koma siniza banvela. 14popeza niza ba mwazya naka vuluvulu mumaziko yonse yamene bakalibe kuonapo, ndiponso malo yazankala yosankaliwamo kuchoka beve. popeza kulibe azapitamalo mumalo olo kubwelelamo pakuti bantu basandusa malo yao yabwino yo onongeka."

Chapter 8

^{1 2 3} mau ya YEHOVA wa makamu yana bwela kuli ine, 2"YEHOVA wama kamu akamba ichi: nili nako kukondesesa pali ziyoni naku kukulu ndiponso nimukondesesa na ukali ukulu! 3YEHOVA wamakamu akamba ichi: niza bwelela kuli ziyoni ndiponso nizankala pakati pa yelusalema, pakuti yelusalema azaitaniwa muzinda wa chilungamo na pili ya YEHOVA wamakamu izaitaniwa pili yoyela! ^{4 5} 4YEHOVA wamakamu akamba ichi: ba nkote ba muna na ba nkote bakazi baza pezeka futi mu tunjila twa yelusalema, ndiponso ali yense muntu aza funika nkoli mumanja yake chifukwa akota maningi. 5tunjila twamumizinda tuzazula banyamata na ba sikana. ⁶ ^{7 8} 6YEHOVA wa makamu akamba izi: ngati chinango chioneka kusa kwanilisika mumenso ya bosala ba bantu bake muma siku yaja, chioneke futi chosa kwanilisika mumenso yanga?-uku nikukamba kwa YEHOVA. 7YEHOVA wama kamu akamba ichi: ona, nili pafupi na kupulumusa bantu banga kuchokela ku ziko ya kunyamuka kwa kazuba ndiponso kuchoka kuziko ya kungena kwa kazuba! 8popeza niza babweza, ndiponso ba zankala pakati pa yelusalema, mwa ichi futi bazanlala bantu banga, na ine nizankala MULUNGU wao muchilungamo na mucha zoon! ^{9 10} 9YEHOVA wa makamu akamba ichi: imwe bamene manje mupitiliza kumvela mau yamozi na yamozi yamene yana bwela kuchoka mukamwa mwa ba neneli' pamene maziko ya nyumba yanga yana ikidwa- iyi nyumba yanga, YEHOVA wama kamu: limbisani manja yanu kuti tempele imangiwe. 10popeza masiku yaja yakalibe kubwela kulibe va mumunda vili vonse vina kololewa nna aliyense, kunalibe kupindula kumuntu olo nyama, ndiponso kunalibe mutendele kuchoka ba dani ku aliyense wo yenda kapena kubwela. nenze nina ika muntu wonse ku ukila munzake. ^{11 12} 1koma manje sichiza nkala monga masiku ya kudala, nizankala nabo bosala ba bantu aba-uku nikukamba kwa YEHOVA wama kamu. 12 popeza mbeu za mtendele ziza shangiwa: mutengo wa mpesa wo kwela pa mwamba uza pasa vi paso vake na ziko iza pasa vo limiwamo; mulenga lenga uza pasa mame yake, popeza niza panga bosalako ba bantu aba kutenga choloba voonse vintu ivi. ^{13 14 15} 13 wenze wo onelako kuli maz iko yena ya tembelelo, nyumba ya yuda na nyumba ya isiraeli. mwa ichi niza kupulumusa ndiponso uzankala mudaliso. usayope: leka manja yako yankale yolimba! 14pakuti YEHOVA wa makamu akamba ichi: monga mwamene nenzo ganizila kukuchita voipa pamene makolo yako yana vundula ukali wanga-akamba YEHOVA wa makamu-- ndiponso sana siye, 15mwa ichi futi niza ganiza mumasiku aya kuchita vabwino futi kuli yelusalema na nyumba ya yuda! usayope! ^{16 17} 16ivi ndiye vintu vamene uyenela kuchita: kamba va zoon, ali yense muntu na munansi wake. waluzi na na chazoon, chilungamo, na mutendele muvipato mwanu. 17musaganize kuchitilana voyipa mukati mwamitima mwanu, ndiponso osakonda kulumbila boza-pakuti ivi ndiye vintu vamene nizonda! uku nikukamba kwa YEHOVA." ^{18 19} 18ndipo mau ya YEHOVA wamakamu ya nabwela kuli ine , kukamba, 19"YEHOVA wamakamu akamba ichi: kusala kudya kwa mumwezi wa 4, mwezi wa 5, mwezi wa 7, na mwezi wa 10 izankala ntau ya chimwemwe, chisangalalo na kukondwela kwa madyelelo pa nyumba ya yuda! mwa icho kondani chazoon na mutendele! ^{20 21 22} 20 YEHOVA wamakamu akamba ichi: bantu bazabwela futi, olo abo bamene bankala mumizinda yambili yosiyana siyana. 21bantu ba mumuzinda winango bazayenda kumuzinda winango na kukamba, 'tiyeni musanga musanga tikapempe pa menso pa YEHOVA na kusakila YEHOVA wamakamu! na ise teka tiyenda. 'bantu bambili na mayiko ya mpamvu bazabwela kusakila YEHOVA wamakamu mu yelusalema na kupempa kukomeledwa mutima kwa YEHOVA! ²³ 23 YEHOVA wamakamu akamba ichi: mumasiku yamene ayo bantu 10 kuchokela ku mitundu yonse na maiko baza gwililila mukanjo wako na kukamba, 'tiyende na iwe, pakuti tamvela kuti MULUNGU ali na iwe!'"

Chapter 9

^{1 2} uku ni kukamba kwa YEHOVA mau pali ziko ya hadaraki na damasiko, malo yake yo pumulilapo; popeza menso ya muntu onse na mitundu yonse ya isilayeli yali pali YEHOVA . Zuku kukamba futi nikwa hamati, wamene malile yake yali pali damasiko, ndiponso kukuza tiro na sidoni, pakuti niba nzelu maningi. ^{3 4} 3tiro azimangila chipupa cholimba na ku unjika siliva monga muchanga na golide yo sungunuliwa monga matika mu tunjila. 4yangana! AMBUYE aza mupoka chuma na kuononga mpamvu yake pa nyanja, mwa ichi aza onongeka na mulilo. ^{5 6 7} 5ashikeloni azaona na kumvela manta! gaza na eve aza tutuma maningi! ekeroni, chiyembekezo chake chizabwezewa pansi! mfumu iza onongeka mu gaza, na ashikeloni saza nkaliwamo futi! 6 bobwela chabe baza panga manyumba yao mu ashidodi, ndiponso niza juba kuzi tukumula kwa ba filisiti. 7popeza niza chosa magari pa kamwa na maloza yao kuchoka pakati pa meno yao. mwa icho bazankala bosalako ba MULUNGU watu monga mutundu mu yuda, na ekironi azankala monga ba yebusi. ⁸ 8 nizankala kuzinguluka ziko yanga kuichingiliza kubankondo baba dani banga, kuti pasankale opitamo kapena kubwelela, kulibe otitikiza amene azaba gonjesa, pali manje ni ona na menso yanga! ^{9 10} 9punda na chisangalalo chikulu, mwana mukazi wa ziyoni! punda na kukondwela, mwana mukazi wa yerusalema!ona! mfumu yako ibwela kuli iwe na chilungamo ndiponso akupulumusa. niwozichepesa ndiponso akwela pa kavalo, pali kamwana ka kavalo. 10 ndipo nizajuba ma galeta kuchoka ku efuremu na ma kavalo kuchokela ku yelusalema, na uta yankondo iza jubiwa kuchoka pa nkondo; pakuti azakamba mtendele pa mayiko, ndiponso ulamulilo wake uzankala kuchoka ku nyanja kuyenda ku nyanja inango, ndiponso kuchoka ku mumana kuyenda kwamene kupela ziko! ^{11 12 13} 11 koma iwe, chifukwa cha magari ya pangano yanga na iwe, niza chosa ba mundende bako mu chimugodi mulibe manzi. 12bwelelani ku linga yanu yolimba, ba mundende ba chiyembekezo! nangu lelo ni kamba kuti niza bwelela kuli imwe kabili, 13popeza na bendeka yuda monga uta yanga. na zulisa----- na efuremu. bana bako bamuna ziyoni na ba ikamo ukali omenyana na bana bako bamuna, greece, ndiponso na panga iwe, ziyoni, ngati lupanga ya wankondo!" ^{14 15} 14 YEHOVA azaonekela kuli beve, ndiponso mivi yake iza lasa monga kaleza! chifukwa chakuti mbuye wanga YEHOVA aza liza lipenga na kufendela na chimpepo kuchoka ku temani.15YEHOVA wamakamu aza ba chingiliza, ndiponso baza baononga na kugonjesa myala zoponyewa. ndiponso bazamwa na kupunda monga bantu ba kolewa na vinyo, ndiponso baza zula na vinyo monga -----, makona ya guwa. ^{16 17} 16 pa siku ija YEHOVA MULUNGU wao az ba pulumusa, monga nkosa za bantu bake. ndiye vobekabeka va chisote cha ufumu vamene viza yaka pa ziko yake. 17 baz wama na kuoneka bwino! ba nyamata baza pukila pa tiligu na ba namwali pa vinyu yo nzuna!"

Chapter 10

^{1 2} pempani mvula kuli YEHOVA mu ntau ya tumvula tung'ono-YEHOVA wamene apanga makumbi ya mvula-ndiponso apasa tumvula towaza kuli aliyense na va masamba mu minda. 2pakuti mafano ya munyumba yamakamba boza; obwebweta alosa va boza; ba makamba maloto ya boza na kupasa chitontozo chilibe kantu, bango yenda yenda monga nkosa na kuvutika chifukwa kulibe mubusa. ³ 3"mukwiyo wanga ukupya pali azi busa; ni mbuzi zi muna - basogoleli- bamene niza pasa chilango. YEHOVA wamakamu aza samala futi nkosa zake, nyumba ya yuda, na kuba panga monga kavalo wa nkondo mu nkondo! ^{4 5} 4mu yuda muzachoka mwala wapangodya; muli eve muzachoka-----; muli eve muzachoka uta ya nkondo; muli eve muzachoka musogoleli aliyense. 5bazankala monga bankondo bamene badyakadyaka badani mumatika ya munjila mu nkondo; baza chita nkondo,pakuti YEHOVA ali na beve, ndiponso baza mvesa nsoni abo bamene baendela pali bakavalo bankondo. ^{6 7} 6 niza limbisa nyumba ya yuda na kupulumusa nyumba ya yosefe,, nizaba bweza na kuba chitila chifundo. bazankala monga kapena sininaba tayepo, pakuti ndine YEHOVA MULUNGU wao, ndiponso nizaba yanka. 7ndiponso Aefuremu bazankala monga ba nkondo, ndiponso mitima zao zizasangalala monga nichifukwa cha vinyo; bana bao baza ona na kusangalala. mitima yao izasangalala muli ine! ^{8 9 10} 8niza balizila mutolilo na kuba ika pamozi, ndaba nizaba pulumusa, ndiponso bazankala bo chuka monga mwamene benzelili kudala! 9nina bamwasya pakati pa bantu, koma bazanikumbukila mumayiko ya mutali mutali, ndipo beve na bana bao baza bwelela nakunkala.10pakuti nizaba bweza kuchoka muziko ya ejipito na kuba unjika pamozi kuchoka ku siriya. nizaba bwelesa muziko ya giliyadi na lebanoni kufikila malo yasile. 11nizapita mu nyanja ya mazunzo yao; niza menya vi mpepo va nyanja yamene iyo naku yumika panyansi nyansi pa mumana wa naile. kuzikuza kwa asiliya kuza bwezewa pansi, ndipo ndodo ya ufumu ya ejipito iza chokapo pali ba ejipito. 12 niza ba limbikisa muli ine neka, ndiponso bazayenda muzina yanga-uku nikukamba kwa YEHOVA

Chapter 11

^{1 2 3} segula viseko vako lebanoni, kuti mulilo uwononge mikunguza yako! 2lilani, mitengo ya paini, pakuti mitengo ya mikunguza yagwa! venze va ulemelelo vaonongeka! lilani, -----pakuti sanga yampamvu yaenda pansi. 3azibusa apunda, pakuti ulemelelo wao wa onongeka! ma liwu ya tunkalamu tun'gono' ya uluma, pakuti ubwino wa yolodani wa onongeka! ^{4 5 6} ndiye chamene YEHOVA mulungu wanga akamba, "monga mubvusa, yanganila nkosa zamene za ikiwa pambali kuti zipayiwe! {bamene bazigula bazipaya elo sibalangiwa, ndiponso bamene b amene bazigulisa bakamba , 'adalisike YEHOVA! nalemela!' pakuti azibusa bosebenezela nkosa' benebake balibe chifundo nazo.6pakuti siniza nvelela futi chifundo bonkala mumalo! - uku nikukamba kwa YEHOVA. ona! ine mwine wake neka nili pafupi nakupindamula muntu ali yense mumanja ya wamene ankala naye pafupi ndiponso mumanja ya mfumu wake, ndiponso baza ononga malo ndipo kulibe aliyense pali beve wamene nizapulumusa kuchoka mukwanja yao," ^{7 8 9} nipo ninankala mubusa wa nkosa zenze kufuna kupayiwa, kuli abo benze kusebenza na mbelele. nina tenga nkoli zibili; nkoli imoza nina yi itana "kukomelewa mutima" ndi[o inango nina yi itana mugwilizano." muli iyi njila nina betela nkosa. 8 mumwezi umozi nina ononga bazibusa batatu. ninankala nilibe chiyembekezo na beve, nabeve bananizonda. 9ndipo ninakamna kuli bene," siniza kusebenzelani monga mubusa futi.mbelele zamene zikufa-zilekeni zife;mbelele zamene zi onongewa-zilekeni zi onongewe. lekani mbelele zamene zisala ili yonse idye tupi ya munzake wa pafupi." ^{10 11 12} ndipo nina tenga nkoli yanga" kukomela mutima" naku ityola kupwanya chipangano chamene nenze ninapanga na mitundu yanga yonse. 11 pa siku ija pangano ina pwanyiwa, ndiponso abo bamenebana sebenzela ku mbelele ndipo benze kuni tamba banaziba kuti YEHOVA akamba. 12 ninakamba kuli beve, "ngati chakuwamizane, nilipileni malipilo anga. koma ngati simufuna, musani pase."ndipo bana pima malipilo anga--siliva zokwanila makumu yatatu. ^{13 14} 13ndipo YEHOVA nakamba kuli ine, "ika siliva mosungila ndalama, mutengo wapamwamba wamene bakuikapo iwe!" ndi[o ninatenga makumi ya tatu ya siliva ija naku peleka mosungila ndalama mu nyumba ya YEHOVA. 14 ndipo nina gomola nkoli yang yachibili, "mugwilizano," kupwanya chibale pakati pa yuda na isilayeli. ^{15 16} YEHOVA anakamba kuli ine, "futi. zitengele vosebenzela va mubusa wopusa, 16 ona, nili pafupi na kuyika mumalo mu busa muziko. saza samalila nkosa zamene zi onongeka. saza yenda kusakila nkosa zamene zasoba, kapena kupolesa nkosa zolemala. saza dyesa nkosa zili na ntanzi, koma azadya nyama ya nkosa zoyina ndipo azazi ng'mba nga'mba. ¹⁷ 17soka kuli mubusa wosila nchito wamene atayilila nkosa! lekani panga ibwele ijube kwanja yake na linso yake yaku kwanja ya manja! lekani kwanja yake ifote na linso yake yaku kwanja ya manja ipofule!"

Chapter 12

^{1 2 3} 1uku nikukamba kwa YEHOVA mau pali isilayeli-kukamba kwa YEHOVA, wamene ana tambasula myamba nakuyanzika maziko ya ziko lapansi, wamene ana wamisa muzimu wa umuntu mukati ka muntu, 2"yangana nili pafupi nakupanga yelusalema kunkala cho mwelamo cholengesa bantu boonse bomuzunguluka kuzezeleka zezeleka. chizankala chimozi mozi kuli yuda pa ntau ya nkonkondo yamu yelusalema. 3pa siku ija niza panga yelusalema mwala wolema pa bantu bonse. ali yense woyesa kunyamula chimwala icho azazichita maningi, ndiponso yoonse maziko ya ziko yaza ungana kuchita nkondo pali muzinda uja. ^{4 5} 4 pasiku ija- uku nikukamba kwa YEHOVA- niza tila musokonezo pali kavalo aliyense nawoikwela niza mufuntika. pali nyumba ya yuda niza segula menso yanga, koma akavalo ba bantu bonse niza bamenya na umpofu. 5ndipo asogoleli ba yuda baza kamba mumitima yao, bantu bamu yelusalema ndiye mpamvu zatu chifukwa cha YEHOVA wa makamu, MULUNGU wao. ⁶ 6pasiku ija basogolelei ba yuda niza bapanga munga mapoto yokupya pakayi pa nkuni ndiponso munga nyali ili imilile pakati pa tiligu, pakuti baza shoka bantu bonse bomuzungulila ku zanja lamanja yao naku mazele. yelusalema azankala futi mumalo yake eka." ^{7 8 9} 7YEHOVA aza yambilila kupulumusa misasa ya yuda, kuti ulemu wanyumba ya davide na ulemu wa abo bonkala mu yelusalema usakulise kuchila bonse bamu yuda. 8pasiku ija YEHOVA azankala ochingiliza wa bonkala mu yelusalema, ndiponso pasiku ija bofoka pakati pao bazankala munga davide, pamene nyumba ya davide izankala munga MULUNGU, munga mungeli wa YEHOVA kusogolo pao. 9pasiku ija yamene niza ononga maziko yonse yamene yachita nkondo na yelusalema. ^{10 11} 10koma nizatila muzimu wachifundo na kupapatila pali nyumba ya davide na bonkala mu yelusalema, baza nililila, munga mwamene winango amalilila mwana mwamuna umozi yeka; bazamulilila mobaba munga bamene balila imfa yamwana mwamuna woyamba. 11pasiku ija kulila mu yelusalema kuzankala munga kulila ku hadadi rimoni mu chigwa cha megido. ^{12 13 14} 12ziko izalila malilo, mutundu uli onse kupatuka kumitundu inango. mutundu wa davide uza patuka na bazikazi bake baza patuka pa bamuna. mutundu wa natani uza patuka na bazikazi bake baza patuka pa bamuna. 13mutundu wa levi uzankala pa weka na bazikazi bake baz patuka kuchoka pa bamuna. mutundu wa simei uzankala pa weka na bazikazi bake baza patuka pa bamuna. 14mutundu uli onse pa mitundu yosalako-mutundu uli onse uzankala paweka na bazikazi bazapatuka pa bamuna."

Chapter 13

^{1 2} pasiku ija manzi aza seguliwa pali nyumba ya davide na bonkala mu yelusalema, pa machimo yao na kusayela kwao. 2 pasiku ija-uku nikukamba kwa YEHOVA wa makamu-niza juba ma zina ya vipembezokuchoka paziko ndiponso siyazaka kumbukiwa futi. niza chosapo baneneli na mizimu ya kusayela pa ziko. ³ ngatu ali onse muntu apitiliza kunenela, atate na amai bana mubala baza mu uza,'si uzankala, pakuti ukamba boza muzinA ya YEHOVA!' ndipo atate na amai bana mubala baza mulasa aka nenela. ^{4 5 6} 4 pasiku ija muneneli aliyense azamvela nsoni na manso mpenya yake akafuna kunenela. aba baneneli sibaza vala futi nkoloko ya usako, kuchitila kuti baname bantu. 5ndaba aliyense azakamba,'sindine muneneli! ndine muntu amene asebenza pa doti, pakuti ntaka ndiye inankala chinto yanga pamene nenze munyamata 6koma wina azakamba kuli eve, 'nivachani vilonda vili pakati pa manja yako?' ndipo azayanka, 'ninachitiwa nabamene bali munyumba yaba nzanga.'" ⁷ " lupanga! kalipila mubusa wanga, bamuna bamene ba imilila pafupi na ine- uku nikukamba kwa YEHOVA wa makamu. menya mubusa, na nkosa ziza mwazyikana! popeza niza nyamula kwanja yanga pali ba pansi pansi. ^{8 9} 8ndipo ivi viza chitika mumalo yoonse- uku nikukamba kwa YEHOVA-----iza jubiwa! baja bantu baza sila kuonongeka; chabe -----ndiye izasalamo. 9nizabwelesa-----mumulilo na kuyisungunula monga siliva imasungunuliwa; niza bayesa monga golide imayesewa. bazayitana pa zina yanga,ndipo nizabayanka nakukamba kuti, 'aba nibantu banga!' ndipo bazakamba, 'YEHOVA ni MULUNGU wanga!'"

Chapter 14

^{1 2} 1onani! siku ya YEHOVA ibwela pamene vintu vonse munapokewa viza gabaniwa pakati panu. 2popeza nizasonkanisa maiko yonse nakumenyana na yelusalema munkondo ndiponso namuzinda uza tengewa. manyumba yaza tengewa na bazimayi baza chitiwa chigololo mokakamiziwa. pakati na pakati pa muzinda bantu baza tengewa ukapolo, koma benangu bantu bazasala sibaza chosewa mumuzinda. ^{3 4} 3koma YEHOVA aza choka nakuyenda ku usha nkondo monga mwamene ana ushila bkondo pasiku yankondo. 4pasiku yamene iyo kwendo yake iza imilia pa pili ya olivi, yamene ku mbali ya yelusalema ku mawa. pili ya olivi iaza gabikana pakati ku maba na kumupoto na chiga chikulu kulu ndiponso pakati pa pili izabwela pafupi na kumupoto inango pafupi na kumwela. ⁵ ndiponso muzatabila kunyansi kwa chigwa pakati pa mapili ya YEHOVA popeza chigwa chili pakati pa mapili ayo chizafika ku hezeli. muzataba monga mwamene muna tabila chivomezi mumasiku ya uziya, mfumu ya yuda. ndipo YEHOVA MULUNGU wanga azabwela na boyela bazankala naye. ^{6 7 8} 6pasiku yamene ija kuzankala kulibe kuwala, ndipo sikuza zizila kapena kupya. 7pasiku yamene iyo, siku yozibika chabe na YEHOVA, kuzankala kulibe muzuba olo usiku, pakuti mumazulo izankala ntau ya kuwala. 8 pasiku iyo manzi ya moyo yaza choka mu yelusalema. yenago manzi yaza kunkulukila ku nyanja ya kumawa ndiponso yenango ku nyanja ya kumupoto, muntawi yakupya na yozizila. ^{9 10 11} 9YEHOVA azankala mfumu pa ziko yonse ya pansi. pasiku iyo kuzankala YEHOVA, MULUNGU umozi, na zina yake eka chabe. 10malo yonse yazankala monga arabala. waku geba kuyenda ku rimona kumupoto kwa yelusalema. yelusalema azapitiliza kunyamuliwa pamwamba mumalo yake eka, kuchoka ku vipata va benjameni kuyenda kumalo kwamene chipata choyamba chinzelili, kuyenda ku chipata cha pokonekela, ndiponso kuchoka ku-----, 11bantu bazankala mu yelusalemandipo kuzankala kulibe chionongeko chosililatu pali beve kuchokela kuli MULUNGU.yelusalema azankala mumutendele. ^{12 13} 12 aya ndiye mavuto yamene YEHOVA azazunza nao bantu boonse bamene benze bana chita nkondo na yelusalema: matupi yao yaza ola koma bali imilile. menso yao yaza ola na malilime yao mukamwa yaza ola. 13pasiku ija manta yakulu yochokela kuli mulungu yaza bwela pakati pao. ali yense aza imilika kwanja ya munzake, ndipo kwanja ya umozi izanyamukila kwanja ya winango. ^{14 15} 14yuda na eve azamenyana na yelusalema. baza sonkanisa chuma cha mayiko yoonse yo bazunguluka- golide, siliva, na vovala va bwino vambili mbili. 15matenda yaza bwela futi pali bakavalo na mabulu, -----,ndiponso pa vinyama vili vonse mumisasa vizadwala matenda yamozi. ^{16 17 18} 16ndiponso ntau yamene iyo kuza pezeke kuti mu maiko yamene yenze ku usha nkondo kuli yelusalema yave yazayamba kuyenda kuchoka chaka pa chaka kuyendo lambila mfumu, YEHOVA wa makamu, ndiponso kusunga pwando ya misasa. 17chizapezeke kuti ngati aliyense kuchokela mu maiko yoonse yapa ziko lapansi sana yende kukwezeka ku yelusalema kuyendo lambila mfumu, YEHOVA wa makamu, ndipo YEHOVA saza leta nvula pali beve. 18 ngati maiko yaku ejipito saza kwezeka kumwamba, ninshi sibaza landila mvula. ntenda kuchokela kuli YEHOVA izagwela maiko yonse yamene siya kwezeka kusunga pwando ya misasa. ¹⁹ 19ichi ndiye chizankala chilango cha ejipito ndiponso chilango cha ziko ili yonse yamene siiza kwezeka kuyenda kusunga pwando ya misasa. ^{20 21} 20koma pasiku ija, ma belo ya akavalo yaza kamba, "kupatiwa kwa YEHOVA," ndiponso ma dishi munyumba ya YEHOVA yazankala monga mbale za pa guwa. 21popeza mpoto iliyonse mu yelusalema na yuda izapatuliwa kuli YEHOVA wa makamu ndiponso ali yense wobwelesa nsembe azadyelamo nakupikilamo. pasiku ija bochita malonda sibazakapezeke futi munyumba ya YEHOVA wa makamu.

Malachi

Chapter 1

¹ ku ukusa kwa mau ya Yehova kupitila muli Malakai. ² "Naku kondani," atalo Yehova. Koma imwe mufunsa kuti, "Mwati konda is?" "Kansi Esau sanali mubale wa Yakobo?" afunsa Yehova. "Koma nakonda Yakobo, ³ ndipo nazonda Esau. napanga lupili yake yosi iwa, na choloba chake malo monkhala magalu ya musanga." ⁴ Ngati Edom akamba kuti, "Tamenyewa, koma tizamanga futi vophwanywa," Yehova wama kamu azakamba kuti, "Banga mange futi, koma niza vigwesa futi. Bazaba itana kuti 'Ziko ya oipa' na 'Banthu bamene mulungu anatembelela muyayaya.'" ⁵ Menso yanu yaza ona ichi, ndipo muzakamba kuti, 'Yehova nimukulu kupitilila malile ya Israeli.'" ⁶ Mwana mwamuna elemekeza batate bake, na wanchito alemekeza bwana wake. Ngati ine, manje, ndine tate, kulemekezewa kwanga kuli kuti? Afunsa Yehova wamakamu kuli imwe bansembe, bamene muchepesa zina

yanga. "Koma mufunsa kuti, 'Tachepesa bwanji zina yanu?' ⁷ Muku pasa buledi yosa enela paguwa yanga. koma funsa, 'Kansi taku pasani bwanji vosa enela?' Chifukwa muyesa guwa ya Yehova ni yosa enela ulemu. ⁸ Ngati mupasaila nyama zilibe menzo ati nsembe, siku ipa uko? Ngati mupeleka volemala na vodwala, siku ipa uko? Vipelekeni kuli bolamulila banu! Azakuvomelani nagu azanya mula nkhope yany?" atelo Yehova wamakamu. ⁹ Manje mu pempha nkhope ya Mulungo, kuti atichitile chisomo, Koma Yehova wamakamu akamba kuti na chopeleka monga ichi mumanja, mwanu, anga nyamule bwanji nkhope ya aliense pali imwe? ¹⁰ "Ngati chabe penze umozi pali imwe wamene angavale viseko va tempele, kuti mu sayashe mulilo paguwa yanga mwachabe! Simuni mvesa bwino," akamba Yehova wama kamu, "ndipo siniza vomela chopeleka chilichonse kuchoka kumanja yanu." ¹¹ Chifukwa kuyambila kuchoka kwa zuba mpaka kunkgena kwake zina yanga iza nkhalala ikulu pakati pa maiko na malo yonse kwemene nsembe na chopeleka cho yela viza pasiwa muzina yanga. Chifukwa zina yamga izankhalala ikulu pakati pamaiko," akamba Yehova wa makamu. ¹² "Koma muinyoza pamene mukamba kuti thebo ya Ambuye niofipisiwa, nakuti vipaso vake, vakudya vake, niva chabechabe. ¹³ Mukamba futi ati, 'Vilemesana ivi,' muimya na mphuno pali ichi," akamba Yehova wa makamu. "Muleta vogwiliwa na nyama zamusaknga nangu volemala nagu vodwala; na kuleta ivi ati chopeleka chanu. Nivomele ivi kuchokela kumanja yanu?" afunsa Yehova. ¹⁴ "Onyenga atembelelewe wamene ali na nyama imuna na kulapila kuipasa kuli ine, koma apasa nsembe ine, Mbuye, vemene sivili bweno! Chifukwa ndine mfumu ikulu," akamba Yehova wa makamu, "na zina yanga izalemekezewa pakati pa maiko."

Chapter 2

¹ Manje imwe bansembe, iyi lamulo niyanu. ² "Ngati simuza mvela, naku chi ika pamutima wanu kuti mupase ulemu kuzina yanga," akamba Yehova wama kamu, "niza tuma tembelelo pali imwe, ndipo nizatembelela daliso yanu. Zoona, naba tembelela, chifukwa simuika lamulo yanga pa mutima wanu. ³ Onani, nili pafupi naku tembelela bana banu, ndipo nizaku zolekani manuwa pamenso, manuwa yochikela ku madyelelo yanu, na ku kutailani pamozi. ⁴ Muza ziba kuti ndine nakutumilani iyi lamulo, nakuti chipangano changa chinga pitilize na Lavi," akamba Yehova wa makamu. ⁵ "Chipangano changa na eve chenzeli cha moyo na mutendele, ndipo nina bapasila kuli eve; nina mupasa mantha, ndipo anani yopa ine, na kuimilila naulemu wazina yanga. ⁶ Malango ya zoona yenzeli mu kamwa mwake, ndipo kulibe boza ilionse yamene ina pezeka pamilomo yake. Anayenda naine mu mutendele nachilungamo naku chosa bambili ku uchimo. ⁷ Chifukwa kamwa ka wansembe kafunika kusunga nzelu na banthu bafunika kusakila malango kuchoka pakamwa pake, chifukwa ni mutumiki wa Yehova wa makamu. ⁸ Koma mwa chokako ku njila ya chilingamo. Mwalengesa bambili ku khumudwa muku konkha lamulo. Mwaphwanya chipangano cha Levi," akamba Yehova wa makamu. ⁹ "Mwa ichi naine, naku pangani bachabe chabe na bomvesa nsoni kubanthu bonse, chifukwa simuna sunge njila zanga, koma mwa onesa kusankha pa malango yanga. ¹⁰ Sikuti kuli tate umozi wa bonse? Si Mulungu wamene anatilenga ise? Nichifukwa chani tilibe chikhulupililo munthu aukila mbale wake, kunyozela chipangano cha azitate bathu? ¹¹ Yuda ankhala alibe chikhulupililo. Chinthu cho nyansa cha chitika mu Israeli namu Yarusalemu. Chifukwa Yuda aipisa malo yoyela ya Yehova yamene akonda, naku kwtila mana mukazi wa mulungu wa chilendo. ¹² Lekani Yehove achose muhema ya Yakobo munthu wamene achita ichi, wamene auka na wamene ayankha, nangu abwelelsa chopeleka kuli Yehova wa makamu. ¹³ Muchita futi ichi: Muvinikula guwa ya Yehova na miszi, na kulila kotaya mutima, chifukwa sayangana ku chopeleka chanu nangu kuchivomela kuchoka mumanja yanu. ¹⁴ Koma mufunsa, "Nichi fukwa chani?" Chifukwa Yehova ndiye mboni pakati kaiwe na mukazi wako wa mu unyamata wako, wamene suna khulupilike kuli eve, nangu enzeli bwenzi na mukazi wako wa chipangano. ¹⁵ Sana bapange umozi, na muzimu wake? Nanga nichifukwa chani anaku pangani umozi? Chifukwa enzofuna chopeleka kuli Mulungu. Mwaicho zichingilize mumzimu, ndipo usankhale osakhulupilika ku mukazi wako wamu unyamata wako. ¹⁶ "Chifukwa nizonda kusila kwa chikwati," akamba Yehova, Mulungu wa Israeli, "na wamene fipisa vovala vake na ndeo," akamba Yehova wa makamu. "Mwaicho zichingilizeni mumzimu wanu ndipo musankhale osakhulupilika." ¹⁷ Mwalemesa Yehova na mau yanu. Koma mukamba kuti, "Tamulemesa bwanji?" Paku kamba kuti, "Aliense wamene achita choipa mumenso ya Yehova, na kukonwela nabo," nangu "Alikuti Mulungu wa chilungamo?"

Chapter 3

¹ "Ona, nili pafupi nakutuma mutumiki wanga, ndipo azakonzeka njila pasogolo panga. Ndipo Ambuye, bamene ufuna, azabwela mwazizizi kutempele yake. Mutumiki wa chipangano wemene usekelelamo, ona, azabwela," akamba Yehova wa makamu. ² Koma ni ndani wamene azakwanisa kupilila siku yakubwela kwake? Nindani wamene azaimilila akaonekela? Chifukwa azankhala monga mulilo wa oyenga na monga sopo yowashila. ³ Azankhala monga oyenga na oyelesa siliva, ndipo aza yelesa bana ba Levi. Azaba yenga monga Golide na siliva, ndipo bazaleta chopeleka cha ulungami kuli Yehova. ⁴ Ndipo chopeleka cha Yuda na Yelusalemu chiza nkhalachokondwelesa Yehova, monga masiku yekudala, na monga muzaka zakudala. ⁵ "Ndipo nizaku konkha kuti niweluze. Niza thamangila kunkhala mbo yosusha mfwiti, bachigololo, baumboni waboza, kusushana na baja bamene banzunza banchito muma lipilo, baja bameme banzunza mukazi ofelewa, na balibe batete bao, kususha na bamene ba pisha mulendo, naba mene sibani lemekeza." akamba Yehova wa makamu. ⁶ "Chifukwa ine, Yehova, sinina chinje; mwaicho imwe bana ba Yakobo, simuna silizike. ⁷ Kuchokela masiku ya bazitate banu mwachokako kumalamulo yanga ndipo simuna yasunge. Bwelelani kuli ine, ndipo niza bwelela kuli imwe," akamba Yehova wa makamu. "Koma mufunsa kuti, 'Tiza belela bwanji?' ⁸ Munthu anga bele Mulungu? Koma muni bela. Koma mufunsa kuti, 'Taku belani bwanji?' Mu chakhumi na chopeleka. ⁹ Ndimwe otembelelewa na tambelelo, chifukwe muni bela, mutundu onse. ¹⁰ Bwelesani chakhumi chokwanila munyumba yosungilamo, kuti munkhale vakudya munyumba yanga, ndipo muniyese manje muli ichi," akamba Yehova wa makamu, "ngati siniza kusegulilani mazenela yaku mwamba nakuthila madaliso pali imwe, mpaka sikuza pezeka malo yoikamo vonse. ¹¹ Niza kamba kusushana nabamene ba baononga mbau zanukuti basaononge kukolola kwa nthaka yanu. Mipesa yanu muminda yanu siza taya vipaso vake," akamba Yehova wa makamu. ¹² "Maiko yonse yazakuitanani odalisika, chifukwa muzankala malo yokondwelesa," akamba Yehova wa makamu. ¹³ "Mau yako yosushana naine yalimbikila," akamba Yehova. "Koma ufunsa kuti, 'Takamba chani pakati pathu chosushana na imwe?' ¹⁴ Wakamba kuti, 'Kulibe phindu kusebenzela Mulungu. Niphindu bwanji kuti tisunge vofunika nagu kuyenda olila pamenso pa Yehova wa makamu? ¹⁵ Apa manje tiitana ba nthota kuti ni bodalisika. Bochita voipa sibaenda chbe pasogolo, koma bayesa na Mulungu na ku thaba. ¹⁶ Ndipo baja bamene beyopa Yehova bakambisana. Yehova anaikako nzelu naku mvela, na buku yachi kumbukilo in lembewa pamenso pake pali baja boyopa Yehova na kulemekeza zina yake. ¹⁷ "Banzankhala banga," akamba Yehova wa makamu, "chuma changa neka chosunga, pasiku yamene nisa chita. Nizaba mvelela chifundo, mongu munthu wamene amvelela chifundo mwana wake wamene amusebenzela. ¹⁸ Ndipo nafuti muza siyanisa pali bolungama na boipa, pakati ka wamene alambila Mulungu na wamene samulambila.

Chapter 4

¹ Chifukwa onani, siku ibwela, yoyaka monga nganjo, pamene opusa na bonse boshita voipa baza sanduka uzu. Siku yamene ibwela izaba shoka," akamba Yehova wa makamu, "mwakuti siiza basilako muzu nangu musambo. ² Koma imwe bamene muyopa zina yanga, zuba ya chilungamo izanyamuka na machiliso muma piko yake. Muzachoka, na kujumpha jumpha monga matole po choka mukhola. ³ Pasiku iyo muza dyaka panzi oipa, chifukwa bazankha mulota pansu pa mapazi yanu pasiku yamene niza chi chita," akamba Yehova wa makamu. ⁴ "Kumbukilani phunziso ya kapolo wanga Mose yamene nina mupasa pa Holebi kuti apase Aisraeli, vokonkha na malamulo. ⁵ Onani, nizakutumilani Eliya muneneli pamene siku ikulu yo yofya ya Yehova ikalibe kubwela. ⁶ Aza chinja mitima ya azitate kuli bana, na mitima ya bana kuli bazitate bao, kuti nisaka bwele na kumenya ziko naku ionongelatu."

Matthew

Chapter 1

¹ Buku ya mubadwe wa Yesu Kristu, mwana wa Davidi, mwana wa Abrahamu. ² Abrahamu anali tate wa Isaki, ndipo Isaki anali tate wa Yakobo, ndipo Yakobo anali tate wa Yuda na babale bake. ³ Yuda anali tate wa Pelezi na Zela kupitila muli Tamar, Pelezi tate wa Hezeloni, ndipo Hezeloni anali tate wake wa Ramu. ⁴ Ramu anali tate wake wa Aminadabu, Aminadabu anali tate wake wa Nashoni, and Nashoni tate wake wa Salimoni. ⁵ Salimoni anali tate wake wa Bowazi kupitila muli Rahabu, Bowazi tate wake wa Obedi kupitila muli Lute, Obedi tate wake wa Yesse. ⁶ Yesse anali tate wake wa Davidi mfumu, Davidi tate wake wa Solomoni kupitila mu mukazi wake wa Yuliya. ⁷ Solomoni anali tate wake wa Rehobowamu, Rehobowamu tate wake wa Abija, Abija tate wake wa Asa. ⁸ Asa anali tate wake wa Yehosafat, Yehosafat anali tate wake wa Yalamu, ndipo Yalamu kolo wa Uziya. ⁹ Uziya anali tate wake wa Jotamu, Jotamu tate wake wa Ahazi, Ahazi tate wake wa Hezekaya. ¹⁰ Hezekaya anali tate wake wa Manase, Manase tate wake wa Amoni, Amoni tate wake wa Josiya. ¹¹ Josiya anali kolo wa Jokoniya na abale bake pa ntawi yo pelekewa ku Babiloni. ¹² Kuchoka ntawi yopelekewa ku Babiloni, Yekoniya anali tate wake wa Shiyatiyewo, Shiyatiyewo anali kolo ya Zelubabewo. ¹³ Zelubabewo anali tate wa Abiyudi, Abiyudi tate wa Eliyakimu, ndipo Eliyakimu tate wa Azo. ¹⁴ Azo anali tate wa Zadoki, Zadoki tate wa Akimu, ndipo Akimu tate wa Eliyudi. ¹⁵ Eliyudi anali tate wake wa Eliyaza, Eliyaza tate wa Matani, ndipo Matani tate wa Yakobo. ¹⁶ Yakobo anali tate wake wa Yosefe mwamuna wa Maria, kupitila mwa eve Yesu anabadwa, wamene aitaniwa Kristu. ¹⁷ Mibadwe yonse kuchokela pali Abrahamu mpaka pali Davidi inali fourteen, kuchokela pali Davidi kufikila ntawi yopelekewa ku Babiloni inali mibadwe 14, ndipo kuchokela ntawi yotengewa ukapolo ku Babiloni kufikila ntawi ya Kristu inali mibadwe 14. ¹⁸ Kubadwa kwa Yesu Kristu kunachitika munjila iyi. Bamai bake, Maria, banakolobekewa kuti bakwatiliwe kuli Yosefe, koma basanabwele pamozi, banamupeza napakati kupitila muli Muzimu Oyera. ¹⁹ Koma Yosefe, mwamuna wake, anali muntu olungama sanafune kuti amuchitile manyazi poonekela, mwa ichi anali kufuna kuti amusiye mwa chisinsi. ²⁰ Pamene eve anali kuganizila ivi vintu, mungelo wa Ambuye unamuonekela eve mu chiloto, nakukamba kuti, "Yosefe mwana wa Davidi, osayopa kutenga Maria kunkala mukazi wako, chifukwa eve wamene apelekewa mwa eve apelekewa na mu Muzimu Oyela. ²¹ Azabeleka mwana mwamuna, ndipo uzamupasa zina Yesu, chifukwa azapulumusya bantu bake kuchoka kuma chimo yao." ²² Ivi vonse vinachitika kuti vifikilise mau yanakambiwa na Ambuye kupitila mwa muneneli, kukamba kuti, ²³ "Taonani, namwali azankala na pakati na kubeleka mwana mwamuna, ndipo bazamuitana zina yake kuti Imanuweli" -yamene tantauzo yake ni, "Mulungu ali naise." ²⁴ Yosefe anauka kuchiloto chake na kucita wamene mungelo wa Ambuye unamuza, nakumutenga kunkala mukazi wake. ²⁵ Koma sanamuzibe kufikila pamene anabeleka mwana wa mwamuna. Ndipo anamuitana zina yake kuti Yesu.

Chapter 2

¹ Pamene Yesu anabadwa mu Betelehemu mu malo ya Yudeya mu masiku ya Helodi mfumu, bamuna bopunzila bochokela ku mawa banafika mu Yelusalemu nakukamba kuti, ² "Nanga alikuti wamene anabadwa Mfumu ya ba Yuda? Tinaona nyenyezi yake ku mawa nichifukwa chake tabwela kumupembeza." ³ Pamene Helodi mfumu anamvela ichi, anavutika mutima, na Yelusalemu yonse. ⁴ Helodi anaitanila pamozi bonse bakulu bansembe na bakalembela ba bantu, naku bafunsa kuti, "Nanga nikuti kwamene Kristu ayenela kubadwila?" ⁵ Bana muuza kuti, "Mu muzinda wa Betelehemu kudela ya Yudeya, chifukwa ichi ndiye chamene chinalembewa na muneneli, ⁶ 'Koma iwe, Betelehemu, mumalo ya Yudeya, sindiwe ochepele pa basogoleri baku Yuda, chifukwa kuchoka kuli iwe kuzabwela olamulira wamene azasogolera bantu banga ba Israyeli. ⁷ Koma Helodi mwachisinsi anaitana bopunzila kuti abafunse ntawi yeni yeni pamene nyenyezi inaonekela. ⁸ Anabatuma ku Betelehemu, kukamba kuti, "Endani muka funisise mwana uyu moikako nzelu. Ngati mwamupeza, nileteleni mau mwakuti naine nibwele nimupembeze." ⁹ Pamene banasiliza kumvela mau ya mfumu, bana enda, ndipo nyenyezi yamene banaona kumawa inabasogolela kufikila pamene inabwela yaimilila pamalo pamene panali mwana wamungono uja analili. ¹⁰ Pamene banaiona nyenyezi ija, banakondwela na chimwemwe chikulu maningi. ¹¹ Banangena munyumba nakumuona mwana mungono anali na Maria mai wake. Banagwa pansi nakumupembeza. Bana masula tuma tumba twabo naku mupasa mpaso za golide, frankincense, na mala. ¹² Mulungu anaba chenjeza muchiloto kuti basabwelele kuli Helodi, chifukwa cha ichi banabwelela ku ziko yabo kusebenzesa njila inangu. ¹³ Pamene bana enda, mungelo wa Mulungu ana onekela kuli Yosefe muchiloto naku muuza kuti, "Uka, tenga mwana mungono na mai wake, tabila ku Igupto. Nkalani kwamene kuja kufikila pamene nizakuuza, chifukwa Helodi azasakila mwana mungono uyu kuti amu ononge." ¹⁴ Usiku wamene uja Yosefe anaoka nakutenga mwana mungono na mai wake naku enda ku Igupto. ¹⁵ Anankala kwamene kuja mpaka kufikila imfa ya Helodi. Ichi china fikiliza vamene Ambuye bana kamba kupitila mumuneneli, "Kuchokela ku Igupto naita mwana wanga." ¹⁶ Koma Helodi, pamene anaona kuti banamunama baja bantu bopunzila, ana kalipa maningi. Anatuma nakupaya bonse bana bamuna bamene banali mu Betelehemu na malo yonse yakuja bamene banali na zaka zibili nakubwela pansi, kukonkeleza ntawi yamene anaganizila pamene anakambisana nabopunzila. ¹⁷ Ichi chinafikiliza vamene vinakambiwa kupitila muli Yelemaya muneneli. ¹⁸ "Liu imveka ku Rama, kulila kwakukulu, Rakeyo ala bana bake, ndiposno akana kutontozewa, chifukwa bana bake basila." ¹⁹ Pamene Helodi anamwalila, onani, mungelo wa Ambuye unaonekela muchiloto kuli Yosefe mu Igupto naku kamba kuti, ²⁰ "Uka tenga mwana na mai wake muyende ku ziko ya Israyeli, chifukwa baja bamene banali kusakila umoyo wamwana bamwalila. ²¹ Yosefe anaima, anatenga mwana na mai wake, naku bwela ku ziko ya Israyeli. ²² Koma pamene anamvela kuti Akelas anali kulamulila mu Yudeya mumalo ya tate wake Helodi, anagwiliwa na manta kuti ayendeko. Pamene Mulungu anamuchenjeza muchiloto, ²³ ana enda kumalo ya Galili naku yenda kukankala mu muzinda oitaniwa Nazaleti. Ichi chinafikiliza chamene chinakambiwa kupitila muli muneneli, kuti azaitaniwa mu Nazaleni.

Chapter 3

¹ Mu ntawi ija Yohane mubatiza anabwela alalikila muchipululu cha Yudeya kuti, ² "Tembenukani, chifukwa ufumu wakumwamba uli pafupi." ³ Chifukwa uyu niwamene anali kukambiwapo na Esaya muneneli, kukamba kuti, "Liu ya muntu wamene aitana muchipululu, 'Konzani njila ya Ambuye, Pangani njila yake yoyondoloka.'" ⁴ Manje Yohane anavala vovala vopangiwa na usako wa Kavalo na beluti mmumazula mwake. Vakudya vake vinali ntete na uchi va musanga. ⁵ Pamene Yelusalemu, yonse Yudeya, na malo yonse yanali kuzungulukila mumana wa Yodani bana enda kuli eve. ⁶ Bana batiziwa kuli enve mumumana ya Yodani, bali kulapa machimo yabo. ⁷ Koma pamene anaona ba Falisi bambili na ba Saduki bali kubwela kuli eve kuti aba batize, anabauza kuti, "Imwe bana ba njoka, nanga nindani wamene akuchenjezani kuti mutabeko ku ukali wamene ubwela?" ⁸ Balani vipaso voyenela kutembenuka. ⁹ Osaganizila kuziiza pakati kanu kuti, 'Tilinaye Abrahamu tate watu.' Chifukwa niku uzani kuti Mulungu akwanilisa ku pasa bana Abrahamu kuchokela ku myala izi. ¹⁰ Apa katemo kaikiwa kudala ku mizyu ya mitengo. Mwa ichi mutengo uli onse wamene siuzapeleka vipaso uzatemewa nakutaiwa mu mulilo. ¹¹ Nikubatzani na manzi ya kutembenuka. Koma wamene abwela pambuyo panga niwamukulu kuchila ine, koma futi na ine sindine oyenela naku nyamula nsapato zake. Azakubatzani na Muzimu Oyela na moto. ¹² Chokololela chake chili mumanja mwake kuti awamye malo opetelapo naku ika pamozi tiligu wake mu nkokwe. Koma azaocha vumvu zonse na moto wamene siunga zimiwe." ¹³ Yesu anabwela kuchoka ku Galili kufika ku mumana wa Yodani kuti abatiziwe na Yohane. ¹⁴ Koma Yohane anayesa yesa kuti amukanile, kukamba kuti, "Ine niyenela kuti nibatiziwe na Imwe, koma Imwe mubwela kuli ine?" ¹⁵ Yesu anamuyanka nakukamba kuti, "Chivomeleze kuti chinkale njila iyi, chifukwa nicho enela kuti tifikilise ulungamo onse." Pamene apo Yohane anamu vomelesa. ¹⁶ Pamene anabatiziwa, Yesu anaimilila mosachedwa kuchoka mumanzi, ndipo taonani, kumwamba kunamu segukila eve. Anaona Muzimu wa Mulungu ubwela pansi monga nkunda naku nkala pali eve. ¹⁷ Onani, liu inabwela kuchokela kumwamba kukamba kuti, "Uyu ni Mwana wanga okondewa. Ndine okondwela naye maningi."

Chapter 4

¹ Yesu anatengewa na Muzimu kuyenda mu chipululu kuti akayesewe na mudyelekezi. ² Pamene anasala chakudya muzuba na usiku masiku yokwanila 40, anamvela njala. ³ Eve oyesa anabwela naku muuza kuti, "Ngati ndiwe Mwana wa Mulungu, uza izi myala kuti zisanduke kunkala mukate." ⁴ Koma Yesu anamuyanka kuti, "chinalembewa kuti, 'Muntu sazankala na moyo kamba ka chakudya cheka, koma na mau yali yonse yamene yachokela mukamwa mwa Mulungu.'" ⁵ Pamene apo mudyelekezi anamutenga kuyenda naye mu muzinda woyela nakumuika pa mwamba mwamba pa tempele, ⁶ naku kumuza kuti, "Ngati ndiwe Mwana wa Mulungu, ziponye pansi, chifukwa nicholembewa kuti, 'Eve azauza bangelo Bake kuti bakusamalile Iwe,' komanso, 'Bazakunyamula mumanja yabo, kuti usamenye kwendo Yako pa mwala.'" ⁷ Yesu anakamba kuli eve, "Futi chinalembewa kuti, 'Usayese Ambuye Mulungu wako.'" ⁸ Futi, mudyelekezi anamutenga pamwamba pa lupili ikulu nakumulangiza ma ufumu yonse yapa ziko yonse pamozi na ulemelelo wao. ⁹ Anamuza kuti, "Vonse ivi vintu nizakupasa Iwe, ngati uzagwada pansi naku nipembeza ine." ¹⁰ Ndipo Yesu anamuza kuti, "Chokapo apa iwe, Satana! Chifukwa chinalembewa kuti, 'Uzalumbila Ambuye Mulungu wako, komanso eve eka ndiye wamene muzatumikila.'" ¹¹ Pamene apo mudyelekezi anamusiya, ndipo onani, bangeli banabwela naku mutumikila. ¹² Manje pamene Yesu anamvela kuti Yohane anagwiliwa, anabwelela kumalo ya ku Galileya. ¹³ Anachokako ku Nazaleti naku yenda kukankala ku Kapenamu, malo yamene yali ku nyanja ya Galileya kumalo yaku Zebuluni na Nafutali. ¹⁴ Ichi chinachitika kuti vamene anakamba muneneli Yesaya vikwanilisike, ¹⁵ "Malo ya Zebuluni na malo ya Nafutali, kuyangana ku nyanja, kupitilila Yodani, Galileya malo yaba Kunja!" ¹⁶ Bantu bamene bankala mumudima baona nchinyali chachikulu, ndiponso kuli baja bamene bankala mumalo komanso mu mfinzi ya imfa, pali beve nyali onekela." ¹⁷ Kuchokela ntawi yamene ija Yesu anayamba kulalikila nakukamba kuti, "Tembenukani, chifukwa ufumu wa kumwamba wabwela pafupi." ¹⁸ Pamene Yesu anali ku enda mumbali ya mumana wa Galileya, ana ona babale babili, Simoni oitaniwa kuti Petulo, na Anduru, mubale wake, banali kuponya chogwililako nsomba mu nyanja, chifukwa banali banthu wogwila nsomba. ¹⁹ Yesu anakamba nabo kuti, "Bwelani, nikonkeni ine, ndipo nizakulengani kunkala bogwila babantu." ²⁰ Pamene apo banasiya vogwililako nsomba naku konka Yesu. ²¹ Pamene Yesu anali kuyenda kuchoka kumalo uku anaona benangu babale babili, Yakobo mwana wa Zebediya, na Yohani mubale wake. Banali mu bwato na Zebediya tate wawo banali kukonza vogwililako nsomba vabo. Anabaitana, ²² pamene apo banasiya bwato na batate babo naku mukonka Yesu. ²³ Yesu anayenda mu Galileya monse, kupunzisa mu ma Sinagogo yabo, kulalikila utenga wabwino wa ufumu, na kuchilisa matenda yosiyana siyana nakudwala pakati pa banthu. ²⁴ Utenga wa eve unayenda konse ku malo ya Siliya, ndipo bantu banamuletela bantu bonse bamene banali na matenda nakubaba kosiyana-siyana, bonse baja bamene bana tengewa na vibanda, bonse ba makate nawonse bolemala. Yesu anabachilisa. ²⁵ Magulu yakulu yanamukonka kuchokela ku malo ya Galileya, Dekapoli, Yelusalemu, na Yudeya, na konse kupitilila Yodani.

Chapter 5

¹ Pamene Yesu anaona magulu, ana enda pa mwamba pa chulu. Pamene anankala pansi, bopunzila bake banabwela kuli eve. ² Anayamba kukamba kubapunzisa, kuti, ³ "Bodalisika nibaja bosauka mumuzimu, chifukwa ufumu waku mwamba niwabo. ⁴ Bodalisika nibaja bamene balila, chifukwa bazatontozewa. ⁵ Bodalisika nibaja bozichepesa, chifukwa bazalandila ziko yapansi. ⁶ Bodalisika nibaja bamane bankala na njala na njota ya chilungamo, chifukwa bazakutisiwa. ⁷ Bodalisika nibaja bachifundo, chifukwa bazalandila chifundo. ⁸ Bodalisika nibaja boyela mutima, chifukwa bazamuona Mulungu. ⁹ Bodalisika nibaja bamane bapanga mutendele, chifukwa bazaitaniwa kuti nibana ba Mulungu. ¹⁰ Bodalisika nibaja bamene banzunziwa chifukwa cha chilungamo, ufumu wa kumwamba niwabo. ¹¹ "Bodalisika ndiwe pamene bantu bakunyoza naku kunzunza naku kamba vosiyana-siyana voipa vaboza pali iwe chifukwa chaine. ¹² Kondwela ndipo nkala nachimwemwe chikulu, chifukwa malipilo yako niyakulu kumwamba. Chifukwa munjila yamene iyi beve bana nzunza baneneli bamene banali ko kumbuyo uku. ¹³ "Ndiwe muchele wa ziko. Koma ngati muchele wasukuluka, unalengewe njila bwanji kuti unkali muchele? Ulibe ntchito iliyonse nafuti koma ku utaya panja naku dyakapo na mendo ya bantu. ¹⁴ Ndimwe ku unika kwa ziko. Muzinda womangiwa pa chulu sungabisiwe. ¹⁵ Kulibe bantu bamene bayasha nyali naku iika pansi pa basketi, koma pa choikapo, ndipo iunikila aliyense munyumba. ¹⁶ Lekani ku unika kwanu ku onekele ku bantu munjila yakuti bangaone zintchito zanu zabwino naku peleka matamando kuli Tate wanu ali ku mwamba. ¹⁷ "Musaganizile kuti ine ninabwelela ku ononga lamulo kapena baneneli. Sinina bwele ku ononga iyayi, koma kufikilisa. ¹⁸ Chifukwa niku uzani kuti ngati chabe kumwamba na pansi kwa sila, kulibe ka lemba kakang'ono kapena ka tito kamene kazachosewamo mu lamulo, mpaka vonse vintu vikakwanilisiwe. ¹⁹ Mwa ichi ali onse wamene apwanya lamulo ing'ono pali aya malamulo nakupunzisa benangu kuchita wamene ivi azaitaniwa mung'ono mu ufumu waku mwamba. Koma ali onse wamene asunga malamulo na kuya punzisa ku bena azaitaniwa mukulu mu ufumu waku mwamba. ²⁰ Niku uzani imwe kuti ngati chilungamo chanu sichizachila chilungamo cha ba kalembela naba Falisi, kulibe njila ili yonse yamene muzaka ngenelamo mu ufumu waku mwamba. ²¹ Munamvela kuti bana uziwa bantu bakudala kuti, 'Usapaye,' futi, 'Ali onse wamene azapaya azankala muchi yopezo cha kuweluziwa.' ²² Koma niku uzani imwe kuti muntu ali onse wamene ankala okalipa na mubale wake azankala muchi yopezo cha chiweluzo; koma futi ali onse wamene auza mubale wake kuti, 'Iwe chimuntu ulibe pindu!' azankala muchi opezo cha ulamulilo; futi ali onse wamene akamba kuti, 'Iwe chipuba!' azankala muchi opezo cha mulilo waku gehena. ²³ Mwa ichi ngati upeleka chopeleka pa guwa koma wabwela wakumbukila kuti mubale wako ali na chinti kumutima chifukwa cha iwe, ²⁴ siya mpaso yako kusogolo ku guwa, enda. Choyamba bwezanani na mubale wako uja, ukasiliza ubwele upeleke mpaso yako. ²⁵ Kambisanani na wamene aku lemba mulandu mwamusanga pamene muli munjila yoyenda kuyi koti, ndaba uja okulemba mulandu azakupeleka kuli oweluza milandu, na uja oweluza milandu azaku peleka kuli musilikali, ndipo munga pelekewe mu ndende. ²⁶ Zoona niku uzani, simuzakachoka mu ndende mpaka mukalipile ndalama zonse zamene muli nazo ngonkole. ²⁷ "Munamvela kuti kunakambiwa, 'Osachite chigololo.' ²⁸ Koma niku uzani kuti bonse bamene balangana mukazi mwa chilakolako balakwa kudala na uja mukazi mu mitima zabo. ²⁹ Ngati linso yako yaku zanja lamanja ikulengesa ulakwe, ichose naku itaya. Chifukwa chawamo kuti mbali imozi ya iwe ionongeke kuchila kuti thupi yako yonse ikataiwe mu gehena. ³⁰ Ngati kwanja yako yaku dzanja lamanja iku lengesa kuti iwe ulakwe, ijube na kuitaya. Chifukwa chawamo kuti mbali imozi ya thupi yako ionongeke kuchila kuti thupi yako yonse itaiwe mu gehena. ³¹ China kambiwa kuti, 'Ali onse wamene apisha mukazi wake, afunika kumupasa kalata yosiliza chikwati.' ³² Koma nikuuzani kuti ali onse wamene asiya muzaki wake, kuchoselako mulandu wa chigololo, amulengesa kunkala wachigololo. Ali onse wamene amukwatila pamene asiya na eve achita chigololo. ³³ "Futi, munamvela kuti chinakambiwa kuli baja bakudala kuti, 'Osalape chaboza, koma upeleke kulapa kwako kwa Ambuye.' ³⁴ Koma niku uzani, musalape nakulapa, kapena kulapila kumwamba, chifukwa ndiye kuli mupando wachifumu wa Mulungu; ³⁵ kapena ziko ya pansi, chifukwa ndiye mupando odyakapo wake; kapena Yerusalemu, chifukwa ndiye muzinda wa Mfumu ikulu. ³⁶ Kapena kulapila mutu, chifukwa sungapange sisi olo imozi yofela kapena yakuda. ³⁷ Koma lekani kukamba kwanu kunkale 'Inde, inde,' kapena 'Iyayi, iyayi.' Chili chonse chopitilila apa chichokela kuli eve oipa. ³⁸ "Munamvela kuti chinakambiwa kuti, 'Linso pa linso, koma futi lino pa lino.' ³⁹ Koma niku uzani imwe kuti, musamukane wamene ni oipa. Koma, ali onse wamene akuchayani ku mbovu imozi, mupaseni akuchayeni naku mbovu inangu iyo. ⁴⁰ Ngati muntu ali onse afuna kuku pelekani ku koti ndipo atenga na chovala chanu, mulekeni uyo muntu atenge na chovala cha pamwamba. ⁴¹ Ali onse wamene akukakamizani kuyenda naye mutunda umozi, endani naye ibili. ⁴² Pasani kuli ali onse wamene akupempani, ndipo musa pilikishe ali onse wamene afuna kukongola kuli imwe. ⁴³ "Munamvela kuti china kambiwa kuti, 'Uyenela kukonda neba wako naku zonda mudani wako.' ⁴⁴ Koma ki uzani kuti, kondani badani

banu ndipo mupempelele baja bamene baku nzunzani, ⁴⁵ mwakuti munkale bana baba Tate banu bamene bali kumwamba. Chifukwa beve bama lenga zuba ku sanika pali baja boipa nabaja babwino, naku tuma mvula pali baja bolungama nabaja bosalungama. ⁴⁶ Chifukwa ngati iwe ukonda chabe baja bamene bakukonda, upezamo chani? Nanga simwamene baja bamusonko bamachitila? ⁴⁷ Ngati mupasa moni chabe babale bane, kansi kusiyana kwanu nabaja benangu kuli pati? Simwamene ba Kunja bamachitila? ⁴⁸ Mwa ichi imwe muyenela kunkala bolungama, monga mwamene balili ba Tate banu baku mwamba.

Chapter 6

¹ "Onesesani kuti simuchita nthito zanu za chilungamo pa menso pa bantu kuti baku oneni, chifukwa simuzalandila malipilo kuchokela kuli ba Tate banu bamene bali kumwamba. ² Pamene mupeleka thandizo, musalinze lipenga monga mwamene baboza bamachitila muma Sinagogo na munjila, mwakuti bangalandile matamando yochoka kuli bantu. Zo ona niku uzani, balandila malipilo yabo. ³ Koma pamene mupeleka thandizo, musaleke kwanja yanu ya kwanja ya manzele izibe chamene kwanja ya manja ichita ⁴ mwakuti mpaso yanu ipelekewe posaonekela. Mwa ichi Tate wanu wamene ali mobisika azakupasani malipilo. ⁵ "Pamene mupempela, musankale monga baja ba boza, chifukwa bama konda kuimilila muma Sinagogo na muma kona mwa njila kuti baonekele ku bantu. Zo ona niku uzani imwe, balandila malipilo yabo. ⁶ Koma imwe, pamene mupempela, endani muchipinda chamu kati. Valani chiseko mupempele kuli ba Tate banu, Bamene bali mobisika. Ba Tate banu bamene baona mu chisinsi bazakupasani malipilo. ⁷ Pamene mupempela, musa kambe mobwezapo bwezapo vilibe na pindu monga ba Kunja mwamene bachitila, chifukwa baganiza kuti bazaba mvela chifukwa cha kupaka kwa mau yabo mu pempelo. ⁸ Mwa ichi, musankale monga beve, chifukwa ba Tate banu baziba vamene imwe mufuna mukalibe naku pempa. ⁹ Mwa ichi pempelani munjila iyi: 'Ba Tate batu bamene muli kumwamba, lekani zina yanu ilemekezeke monga yoyela. ¹⁰ Lekani ufumu wanu ubwele. Lekani kufuna kwanu kuchitike pa ziko monga mwamene chilili kumwamba. ¹¹ Mutipase lelo mukate watu walelo. ¹² Tikululukileni ma chimo yatu, monga mwamene ise tikululukila bamene bati lakwila ise. ¹³ Musatipeleke mu ma yeso, koma mutichose ku oipa.' ¹⁴ Chifukwa ngati imwe mukululukila bantu volakwa vabo, ba Tate banu baku mwamba baza kukululukilani naimwe. ¹⁵ Koma ngati imwe simukululukila volakwa vabo, naimwe ba Tate banu sibazakukululukilani volakwa vanu. ¹⁶ "Pamene muzimana chakudya, musankale na pamenso monga mulila monga mwamene bantu baboza bamachitila, chifukwa bama chinja pamenso kuti baonekele ku bantu kuti ba zimana chakudya. Zo ona ni kuuzani imwe, balandila malipilo yabo. ¹⁷ Koma imwe, pamene muzimana chakudya, zolani mafuta ku mutu musambe na ku menso ¹⁸ kuti musaonekele kuli bantu kuti muzimana chakudya, koma kuli ba Tate banu chabe bamene bali mobisika; ba Tate banu bamene baona mobisika bazakupasani malipilo. ¹⁹ "Musazisungile mweka chuma pa ziko, pamene vidoyo na nguwe imaononga, futi pamene ba kawalala bama ngena naku ba. ²⁰ Koma, zisungileni mweka chuma kumwamba, kwamene vidoyo kapena nguwe si ingaononge, kwamene ba kawalala siba ngangene na kuba. ²¹ Chifukwa kwamene kuli chuma yanu, kwamene uko ndiye kuzankala na mutima wanu. ²² Linso ndiye nyali ya ku thupi. Mwa ichi, ngati linso yanu ili bwino, thupi yanu yonse izankala yozula na ku ngwelebelo. ²³ Koma ngati linso yanu niyo ipa, thupi yanu yonse izankala na mudima. Mwa ichi, ngati nyali yanu yamene ili mukati mwanu ni mfinzi, onani kukula kwa chimudima icho! ²⁴ Kulibe kapolo angasebenzele ba kazembe babili, chifukwa aza zondapo umozi naku konda uja winangu, kapena azazipeleka kuli umozi na kunyozela uja winangu. Simunga tumikile Mulungu na chuma. ²⁵ Mwa ichi ni kuuzani imwe, musankale ovutika pa zau moyo, vamene muzadya kapena vamene muzamwa; kapena pa za thupi, vamene muzavala. Kansi moyo siuchila vakudya, na thupi si ichila vovala? ²⁶ Onani tunyoni twa mumwamba. Situmalima kapena kukolola kuika mu nkokwe, koma Tate wanu waku mwamba amatudyesa. Nanga imwe sindimwe ba mutengo wapa mwamba kuchila tweve? ²⁷ Nindani pali imwe wamene muku pitila movutikila mutima angaikileko ku utali wa umoyo wake? ²⁸ Nanga nichifukwa chani muvutika mutima pali vovala? Ganizilaniponi pali tuma luwa twa mu sanga, mwamene tuma kulila. Situma sebenza, situmatunga vovala. ²⁹ Koma niku uzani imwee kuti, Solomo mu ulemelelo wake onse sana valeko monga tuma luba utu. ³⁰ Ngati Mulungu amavalika ma uzu sanga, yamene lelo yaliko koma mailo yataiwa mu mulilo, kuchilapo njila bwanji mwamene Mulungu azaku valikani imwe, imwe bochepekela chikululupilo? ³¹ Mwa ichi musankale bovutika mutima nakukamba kuti, 'nanga tizadya chani kansi' kapena 'Nanga tizamwa chani kansi?' kapena 'Nanga tizavala vovala viti kansi?' ³² Chifukwa bakunja bamafunafuna ivi vintu, koma ba Tate banu baziba kuti mufunikila ivi vintu. ³³ Koma choyamba funani ufumu waku mwamba na chilungamo chake, ndipo ivi vonse muzapasiwa. ³⁴ Mwa ichi, musankale bovutika mutima pa za mailo, chifukwa mailo iza zivutikila pa yka. Siku iliyonse ilinavo voipa vake yeka.

Chapter 7

¹ Osaweluza, naiwe siuzaweluziwa. ² Chifukwa mwamene iwe uweluzila benangu ndiye mwamene naiwe uzaweluziwa, na mwamene uzapimila chiweluzo chako ndiye mwamene bazakuweluzila naiwe. ³ Nanga nichani ulanganila pa kauzu kamene kali mu linso ya mubale wako koma uibala chi nkuni chamene chili mu linso yako? ⁴ Nanga uzamuuza bwanji mubale wako kuti, 'Leka nikuchose ka uzu kali mu linso yako,' koma chinkuni chili mu linso yako? ⁵ Iwe wa boza! Yambilila kuchosa chinkuni mu linso yako, kuchoka apo ndiye pamene uzaona bwino kuti ukwanisa kuchosa kauzu kali muli linso ya mubale wako. ⁶ Osapasa imbwa vintu voyela, ndipo musaponyele myala zamutengo wapatali pamenso pa nkumba ya musanga. Ndaba vizadyakapo na mendo, nakupindamuka naku kusansaulani imwe. ⁷ "Pempa, ndipo uzapasiwa. Sakila, ndipo uzapeza. Konkosha, ndipo bazakusegulila. ⁸ Chifukwa muntu aliwonse wamene apempa amalandila; aliwonse wamene amasakila, amapeza; na kuli uja wamene akonkosha, bazamusegulila. ⁹ Kaya ngati nindani pali imwe, wamene ngati mwana wake amupempa buledi, azamupasa mwala? ¹⁰ Kapena ngati apempa nsomba, azamupasa njoka? ¹¹ Mwa ichi, ngati imwe boipa muziba kupasa mpaso zabwino kuli bana banu, nanga ba Tate banu bali kumwamba bazakuchitilani bwanji mukupasa vintu vabwino kuli baja bamene baba pempa? ¹² Mwa ichi, chilichonse chamene ufuna kuti bantu bakuchitile iwe, naiwe uyenela kubachitila, aya ndiye ma lamulo na baneneli. ¹³ Ngena kupitila pa chiseko chingono. Chifukwa chiseko na njila ikulu ndiye vamene vipeleka ku chionongeko, ndiponso nibambili bamene ba ngenela mwamene umo. ¹⁴ Koma chiseko nichingono na njila niyovuta yamene ipeleka kuli moyo, ndipo nibangono bamene baipeza. ¹⁵ Nkalani bochenjela naba neneli baboza, bamene babwela kuli imwe bavala vovala va nkosa koma mukati ni mimbulu yanjala ikulu. ¹⁶ Muzabazibila kuvipaso vabo. Nanga bantu bamatyola mpesa ku mutengo waminga kapena mukuyu ku minga? ¹⁷ Munjila imozi-mozi, mutengo onse wabwino umabala vipaso vabwino, koma mutengo oipa umabala vipaso voipa. ¹⁸ Mutengo wabwino siungabale vipaso voipa, kapena mutengo oipa kubala vipaso vabwino. ¹⁹ Mutengo uli onse wamene siumabala vipaso vabwino umatyolewa naku taiwa mu mulilo. ²⁰ Mwa ichi, muzabaziba kupitila muvipaso vabo. ²¹ Simuntu aliwonse wamene akamba kuli ine kuti, 'Ambuye, Ambuye,' wamene azakangena mu ufumu wakumwamba, koma baja chabe bamene bachita chifunilo chaba Tate banga bamene bali kumwamba. ²² Bambili bazakamba kuli ine pa siku ija, 'Ambuye, Ambuye, ife sitinali kupeleka uneneli mu zina yanu, muzina yanu tinali kuchosa vibanda, muzina yanu tinachita vintu vikulu kwambili? ²³ Pamene apa nizakabauza po onekela kuti, 'Sininakuzibeni! Chokani pamenso panga, imwe bamachitidwe yoipa!' ²⁴ "Mwaichi, muntu aliwonse wamene amvela mau yanga na kuchita vamene nakamba azankala monga muntu wamene amanga nyumba yake pa mwala. ²⁵ Mvula inagwa, vimanzi vinabwela, na chimpepo chinaputa na kumenya nyumba ija, koma si inagwe pansu, chifukwa ina mangiwa pa mwala. ²⁶ Koma muntu aliwonse wamene amvela mau yanga koma sachita vamene nakamba ali monga uja muntu opusa wamene anamanga nyumba yake pa muchenga. ²⁷ Mvula inagwa, vimanzi vinabwela, na chimpepo chinaputa na kumenya ija nyumba, ndipo inagwa, na kuonongeka kwake kunali kuja kofikapo. ²⁸ Pamene Yesu anasiliza kukamba aya mau, magulu ya bantu yanadabwa na kupunzisa kwake, ²⁹ chifukwa anali kubapunzisa monga uja muntu wamene ali na ulamulilo, osati monga baja bakalembela.

Chapter 8

¹ Pamene Yesu anaseluka ku pili, magulu ya bantu yanamukonka. ² Onani, muntu wa makate anamukonka na kugwada pansi, nakukamba kuti, "Ambuye, ngati mufuna, mungani polese." ³ Yesu anatambasula kwanja yake naku mugwila, naku kamba kuti, "Nifuna. Pola." Pamene apo eve anapolesewa ku matenda yake ya makate. ⁴ Yesu anamuza kuti, "Onesesa kuti usauze muntu aliwonse kantu. Yenda, kazilangize kuli mukulu wa nsembe, na kupeleka chopeleka chamene Mose anakuuzani, kupeleka umboni kuli beve." ⁵ Pamene anali kubwela ku Kapenamu, mukulu wabasilikali anabwela kuli eve, kumupemba ⁶ nakukamba kuti, "Ambuye, wantchito wanga kunyumba aligone adwala alibe mpavu ndipo amvela kubaba kukulu." ⁷ Pamene apo Yesu anamuza kuti, "Nizabwela nimupolese." ⁸ Eve mukulu wa asilikali anamuyanka nakuti, "Ambuye, ine sindine oyenela kuti imwe mubwele kungenda munyumba yanga. Koma kambani chabe mau wantchito wang aazapola." ⁹ Chifukwa ine ndine muntu wamene ali pansi pa bakulu bantchito, naine nilinabo basilikali pansi panga. Nikamuza umozi kuti, 'yenda,' amayenda, nakuli winangu kuti, 'bwela,' amabwela, nakuli wantchito wanga kuti, 'Chita ichi,' amachita." ¹⁰ Pamene Yesu anamvela ivi, anadabwa nakuza bantu bamene banali kumukonka kuti, "Zona nikuuzani imwe, nikalibe kupezapo muntu aliwonse wamene ali na chikulupililo monga ichi mu Israeli." ¹¹ Nikuuzani kuti, bantu bambili bazakabwela kuchokela kumawa na ku mazulo, ndipo bazankala pamalo podyela pamozi na Abrahamu, Isaki, na Yakobo, mu ufumu wakumwamba. ¹² Koma bana ba mu ufumu bazataiwa panja mumu mudima, kwamene kuzankala kulila na kusheta meno." ¹³ Yesu anakamba kuli uja mukulu waba silikali, "Yenda! Monga mwamene wakulupilila, leka chikuchitikile iwe." Uja wantchito wake anapolesewa pa ntawi yamene ija. ¹⁴ Pamene Yesu anabwela munyumba ya Petulo, anaona bapongozi ba Petulo baligone namatenda ya kupya tupi. ¹⁵ Yesu anagwila kwanja yabo, kupya tupi kunayenda pamene apo. Banaima na nakuyamba kumusebenzela. ¹⁶ Pamene kunankala ntawi yaku mazulo, bantu banaleta kuli Yesu bantu bambili bamene banali na zibanda. Anabachosa vibanda kusebenzesa chabe mau nakupolesa bonse bamene banali namatenda. ¹⁷ Munjila iyi mau yamene yanakambiwa na muneneli Yesaya yanafikilisiwa, kukamba kuti, "Eve eka anatitengela kusamvela bwino kwatu naku nyamula matenda yatu." ¹⁸ Manje pamene Yesu anaona gulu yabantu banamuzungulukila anabauza kuti bachokeko bayenda kumbali ina ya Galili. ¹⁹ Ndipo eve wolemba anabwela kuli Yesu nakukamba kuti, "Mupunzisi, ine nizakukonkani kuli konse kwamene imwe muzayenda." ²⁰ Yesu anamuza kuti, "Nkandwe zili na monkala, tunyoni twa mumwamba tuli nato tuchisa, koma Mwana wa muntu eve alibe na poika mutu." ²¹ Wina pali wopunzila anamuyanka kuti, "Ambuye, nivomeleseni kuti niyende nikashike ba tate banga." ²² Koma Yesu anamuza kuti, "Konka ine, baleke bakufa bashikane beka." ²³ Pamene Yesu anangena mu bwato, bopunzila bake banamukonka. ²⁴ Onani, kunabwela chimpepo chikulu pa nyanja, mwakuti bwato inazula na manzi. Koma Yesu anali akali gone. ²⁵ Bopunzila bake banenda kuli eve na kumuusha, nakumuza kuti, "Tipulumuseni, Ambuye; tifuna kufa!" ²⁶ Yesu anakamba kuli beve kuti, "Nanga nichani muli na manta, imwe bochepe chikulupililo?" Anaima naku kalipila chipempepo na nyanja. Chipempepo chinabwela chasila. ²⁷ Bantu baja banadabwa kwambili nakukamba kuti, "Nanga nimuntu wa bwanji kansi uyu, wamene na chimpepo na nyanja vimumvelela?" ²⁸ Pamene Yesu anabwela kumalo kwina ku ziko yaku ba Gadalene, bamuna babili bamene banali na vibanda banamukumanya eve. Banali kuchokela ku manda ndipo banali ba ndeo, chifukwa chake kulibe muntu wamene anali pa ulendo wamene anali kupitila njila iyi. ²⁹ Onani, banapunda nakukamba kuti, "Nanga nichani chamene ufuna kuli ise iwe, Mwana wa Mulungu? Nanga wabwela kuno kuti utizunzise pamene ntawi yamene inaikiwa ikalibe kufika?" ³⁰ Manje gulu ya nkumba inali kudya, osati kutali maningi na beve. Vibanda vinapitiliza kumupemba Yesu kuti, ³¹ "Ngati mwatichosa, tiuzeni tiyenda muli gulu ya nkumba." ³² Yesu anaviuza kuti, "yendani!" Vibanda vinachoka nakuyenda mu nkumba; ndipo onani, gulu yonse ya nkumba zinataba nakuyenda kuseluka chulu kuyenda mu nyanja mwamene zinafela mumanzi. ³³ Baja bamene banali ku betela nkumba banataba naku enda mu muzinda naku uza bantu vonse vamene vinachitika, maka-maka vamene vinachitika kuli baja bamene banali na vibanda. ³⁴ Onani, muzinda onse unabwela kuti uone Yesu. Pamene banamu ona Yesu, banamupapatila kumupemba kuti achoke ku malo yabo.

Chapter 9

¹ Yesu anangena mu bwato, naku enda kumbali kwina kwa nyanja, nakufika ku muzinda kwake. ² Onani, banamuletela muntu wama manjenje aligone pa mpasa. Pamene anaona chikulupililo chabo, Yesu anamu uza uja muntu, "Mwana, nkala okondwela. Machimo yako yakululukiwa." ³ Onani, benangu pali bolemba banayamba kukamba pabeka kuti, "Uyu muntu anyoza." ⁴ Yesu anaziba maganizo yabo naku bauza kuti, "Nanga nichani imwe muganiza voipa mumitima zanu?" ⁵ Nanga nichiti chintu chamene sichishupa, kukamba kuti, 'Machimo yako yakululukiwa,' kapena kukamba kuti, 'Ima uyende?' ⁶ Koma kuti imwe muzibe kuti Mwana wa Muntu alinayo mpavu pa ziko yo kululukila machimo, ... anakamba ku uza uja wamanjenje kuti, "Imilila, tenga mpasa yako, enda kunyumba kwako." ⁷ Pamene apo mwamuna uja ananyamuka naku enda kunyumba kwake. ⁸ Pamene gulu ya bangtu inaona ivi, banadabwa nakuyamba kutamanda Mulungu, wamene anapasa mpavu zamutundu uyu ku bantu. ⁹ Pamene Yesu anali kupita paga, anaona muntu zina yake Mateyo ali nkale posebenzela baja bamusonko. Anamu uza eve kuti, "Nikonke." Anaima nakumukonka. ¹⁰ Pamene Yesu anankala kuti adye munyumba, onani, bambili ba musonko na bamachimo banabwela nakudya pamozi na Yesu na bopunzila bake. ¹¹ Pamene ba Falisi banaona ivi, banakamba kuli bopunzila ba Yesu kuti, "Nanga kansi nichani chamene bapunzinsi banu badyela pamozi naba musonko na bantu bama chimo?" ¹² Pamene Yesu anamvel aivi, anakamba kuti, "Bantu bamene bali bwino mu mubili sibafunika kuona dotolo, koma baja bamene nibodwala." ¹³ Endani muka punzile tantauzo ya kukamba uku: 'Ine nifunapo kunkala na chifundo kuchilapo nsembe.' Chifukwa ine sininabwele kuitana bolungama kuti batembenuke, koma bamachimo. ¹⁴ Bopunzila ba Yohane banabwela kuli eve nakukamba kuti, "Nanga nichani ise na ba Falisi timazi mana chakudya kambili, koma bopunzila banu beve sibama zimana?" ¹⁵ Yesu anaba yanka, "Nanga bantu boitaniwa ku ukwati banga mvese chifundo pamene okwatiliwa akali nabo? Koma ma siku yazakabwela pamene okwatiliwa azakatengewa, pamene apo bazakazimana chakudya." ¹⁶ Kulibe muntu wamene aika kanyula ka manje pali chovala chakudala, chifukwa kanyul aaka kazangamba chovala, kungambika kweve kuzankala kukulu. ¹⁷ Nafuti bantu sibamaika vinyo va manje mu voikamo vakudala. Ngati bachita ichi, voikamo vizapwanyika, vinyu vizataika, na voikamo vizaonongeka. Koma, bamaika vinyu va manje mu voikamo vamanje, munjila iyi vonse visasungiwa chabe bwino. ¹⁸ Pamene Yesu anali kubauza ivi vintu, onani, kazembe umozi anabwela naku gwada kuli Yesu. Nakukamba kuti, "Mwana wanga mukazi amwalila, koma bwelani mumuika kwanja, azauka." ¹⁹ Pamene apo Yesu anaima naku mukonka, na bopunzila bake na beve banakonka. ²⁰ Onani, mukazi wamene anali na vuto yochoka magari zaka zopitilila kumi ya zibili anabwela kumbuyo kwa Yesu naku gwila kunyansi ya chovala chake. ²¹ Chifukwa anaziuza mukazi uyu eka kuti, "Ngati chabe nagwila vovala vake, Ine nizankala chabe bwino." ²² Koma Yesu anapindimuka naku muona, nakukamba kuti, "Mwana wanga mukazi, nkala olimba, kukulupilila kwako kwaku polesa." Pamene apo uja mukazi anapola. ²³ Pamene Yesu anafika munyumba ya uja kazembe, anaona bolinza mitoli na gulu ya bantu ipanga chongo. ²⁴ Anabauza kuti, "Tiyeni endani, uyu mukazi sanamwalile, koma agona chabe." Koma banamu seka monyezela. ²⁵ Pamene gulu ija inachoka panja, anangena mu chipinda naku mugwila kukwanja, mukazi uja anauka. ²⁶ Nkani ya uyu utenga ina enda mumalo yonse. ²⁷ Pamene Yesu anali kupita kuchokela kuja, bamuna babili bamen banalibe menso banamukonka. Banapitiliza kupunda naku kamba kuti, "Tichitleni chifundo ise, Mwana wa Davide!" ²⁸ Pamene Yesu ananegna munyumba, bamuna baja banalibe menso banabwela kuli eve. Yesu anabauza kuti, "Mukulupilila kuti ninga kwanise ichi?" Bana muyanka kuti, "Inde, Ambuye." ²⁹ Pamene apo Yesu anabagwila pamenso nakukamba kuti, "Lekani chikuchitikileni kulingana na chikulupililo chanu," ³⁰ na menso yabo yanaona. Yesu anabauza mobalimbikisa kuti, "Onani kuti kulibe muntu ali onse wamene azaziba ichi." ³¹ Koma bamina baja babili bana enda naku peleka mau ku malo yonse yakuja. ³² Pamene baja bamuna banali kuenda, onani, mwamuna chiulu wamene anali na vibanda banamuleta kuli Yesu. ³³ Pamene chibanda chinachosewa, uja chibulu anayamba kukamba. Ma gulu ya bantu yana dabwa nakukamba kuti, "Ichi chikalibe kuonekapo mu Islayeli!" ³⁴ Koma ba Falisi beve banali kukamba kuti, "Nichifukwa cha mukulu wa vibanda, ndiye chamene akwanilisila kuchosa vibanda." ³⁵ Yesu anaenda-enda mumizinda na mumenzi yonse. Anapitiliza kupunzisa muma sinagogo yabo, kulalika utenga wa ufumu na kupolesa matenda yamu tundu onse na kusamvela bwino kosiya-siyana. ³⁶ Pamene anaona magulu, anamvela chifundo, chifukwa banali bovitika mitima nafuti bobwezewa kumbuyo. Banali monga nkosa zamene zilibe ozibeta. ³⁷ Anakamba kuli bopunzila bake kuti, "Vokolola nivambili, koma banchito ndiye bamene bachepa." ³⁸ Chifukwa chake imwe muyenela kupempela kuli Ambuye ba vokolola, kuti batume banchito mu munda wabo."

Chapter 10

¹ Yesu anaitana bopunzila bake nakubapasa mpavu pali mizimu za doti, kuti bazivichosa, naku polesa matenda yosiyana-siyana na kusamvela bwino kuli konse. ² Mazina ya bopunzila bali kumi imozi na tubili ni aya. Oyamba, Simoni (wamene anapasa zina yakuti Petulo), na Andulu mubale wake; Yakobo mwana wa Zebedi, na Yohane mubale wake; ³ Filipi, na Batolomeu; Tomasi, na Mateyo uja wamusonko; Yakobo mwana wa Alufeyo, na Tadeyasi; ⁴ Simoni Siloti, na Yudas Isikalioti, wamene anamugulisa. ⁵ Aba bali kumi na tubili Yesu anabatuma. Anabapasa lamulo nakubauza kuti, "Musangene mumalo yali yonse kwamene kunkala ba Kunja, nafuti musangene mu muzina uli onse waba Samalita. ⁶ Koma endani kuli nkosa zotaika za munyumba mwa Islayeli, ⁷ pamene mu enda, mukazilalikila nakukamba kuti, 'Ufumu waku mwamba wabwela pafupi.' ⁸ Polesani bodwala, ukisani bantu bakufa, polesani bali na makate, chosani vibanda. Mwalandila mosalipila, naimwe pasani mosalipilisa. ⁹ Musatenge golide ili yonse, siliva, kapena kopa mu ma tumba yanu. ¹⁰ Musatenge chola pa ulendo wanu, kapena chovala chinangu, kapena nsapato, kapena ndodo, chifukwa wantchito ayenekela kumupasa chakudya. ¹¹ Muzinda uli onse kapena munzi uli onse wamene mwangenamo, pezani wamene ali onela mwamene umo, nkalani mwamene umo mpaka mukachokemo. ¹² Pamene mungena munyumba iyo, pelekani moni. ¹³ Ngati nyumba niyoyenela, lekani mutendele wanu unkale pali yeve. Koma ngati siyoyenela, lekani mutendele wanu ubwelele kuli imwe. ¹⁴ Koma kuli baja bamene sibakulandilani kapena kumvela mau yanu, pamene imwe muchoka munyumba ija kapenam muzinda, chosani doti kumendo yanu. ¹⁵ Niku uzani cha zo-ona kuti, chizainkalilako bwino malo ya Sodoma na Gomola pa siku yoweluza kuchilapo muzinda uyo. ¹⁶ "Onani, Nikutumani monga nkosa pakati pa mimbulu, chifukwa chake nkalani bochenjela monga njoka koma na mutima monga wa nkunda. ¹⁷ Koma nkalani bochenjela na bantu! Bazakupelekani kuli bakulu ba milandu, ndipo bazakumenyani mu ma sinagogo yabo. ¹⁸ Kukonkapo bazakuletani pa menso pa ba Kazembe na mafumu chifukwa cha Ine, kunkala monga mboni kuli beve na kuli bakunja. ¹⁹ Pamene bakupelekani, musankale bovutika mutima pali mwamene muzakambila kapena vamene muzakamba, chifukwa vamene muzafunika kukamba pali ntawi yamene ija muzakapasiwa. ²⁰ Chifukwa sindimwe bamene muzakamba iyayi, koma Muzimu wa Atate banu ndiye wamene azakamba kupitila muli imwe. ²¹ Mubale azakapeleka mubale wake ku imfa, na tate mwana wake. Bana bazaka ukila makolo yabo nakulengesa kuti babapaye. ²² Muzazondewa na bonse chifukwa cha zina yanga. Koma wamene azakalimbikila kufikila kosilizila, uja munt azakapululumuka. ²³ Pamene bazaku vutisani mumuzinda uyu, tabilani ku muzinda winangu, chifukwa niku uzani imwe, simuzaka kwanisa kuyendamo mumizinda za Islayeli zonse Mwana wa Muntu akalibe naku bwela. ²⁴ "Opunzila simukulu kuchila omupunzisa, kapena wanthito achile bwana wake. ²⁵ Chilibwino kuti opunzila ankale monga omupunzisa, na wanchito ankale monga bwana wake. Ngati bana itana bwana wa nyumba kuti eve ni Belezababu, nanga bantu bamu nyumba bake bazaba itana mazina yoipapo bwanji kans! ²⁶ Chifukwa chake imwe musaba yope, chifukwa kulibe kantu kamene nikobisika kamene sikazakaonesewa, nafuti kulibe kamene kali nikobisika kamene sikazazibika. ²⁷ Vamene niku uzani usiku, vikambeni muzuba, na vamene mumvela mobweza mau mu matu, vikambeni pa mwamba pa mutenge. ²⁸ Mosayopa baja bamene bapaya tupi koma sibakwanisa kupaya moyo. Koma, yopani wamene akwanisa kuononga moyo na tupi ku nganjo ya moto. ²⁹ Nanga kans tu nyoni tubili situma gulisiwa pa ka ndalama kamozi? Koma kulibe nangu kamozi kamene kamagwa pans! Atate banu osaziba. ³⁰ Koma naimwe sisi zanu mumutu zonse nizopendewa. ³¹ Musayope. Imwe ndimwe bamutengo wapatali kuchila tunyoni twambili. ³² Chifukwa cha ichi muntu ali onse wamene anivomela pamenso pa ya bantu, naine nizamu vomela pammenso ya Atate banga bamene bali kumwamba. ³³ Koma uja wamene anikana pamenso ya bantu, naine nizakamukana pamenso yaba Tate banga bamene bali kumwamba. ³⁴ "Musaganize kuti ine ninabwela kuleta mutendele pa ziko yapansi. Sininabwelele kuleta mutendele, koma lupanga. ³⁵ Chifukwa ine ninabwela kuika mwamuna kushushana na tate wake, mwana mukazi kushushana na mai wake, na mupongozi mukazi kushushana na bapongozi bakazi bake. ³⁶ Bozonda muntu bazankala bamene baja bamu nyumba yake. ³⁷ Uja wamene akonda batate bake kapena bamai bake kuchila ine sayenela ine; wamene akonda mwana mwamuna kapena mwana mukazi kuchila ine sioyenela ine. ³⁸ Wamene sazanyamula mutanda wake nakuni konka ine sayenela ine. ³⁹ Wamene apeza moyo wake azautaya. Koma wamene ataya moyo wake chifukwa cha ine azaupeza. ⁴⁰ Wamene akulandilani imwe alandila ine, na uja wamene alandila ine alandila eve wamene ananituma. ⁴¹ Wamene alandila muneneli chifukwa ni muneneli azalandila malipilo ya muneneli, na uja wamene alandila muntu wachilungamo chifukwa ni olungama azalandila malipilo ya muntu olungama. ⁴² Ali onse wamene apasa olo chabe manzi yakumwa yozizila kuti amwe mwana wamene ali opunzila wanga, zo-ona niku uzani imwe, sazataya malipilo yake."

Chapter 11

¹ Pamene Yesu anasiliza ku uza bopunzila bake bali 12 vochita, anachokako kuyenda mukupunzisa mumizinda zabo naku lalikila. ² Manje pamene Yohane anamvela pali vamene Kristu anali kuchita, anatumiza mau kupitila muli bopunzila bake ³ kukamba kuti, "Kansi ndiwe wamene ubwela, kapena nangu tiyembekeze winangu?" ⁴ Yesu anabayanka nakukamba kuti, "Yendani mukamuuze Yohane vamene muona navamene munvela. ⁵ Mpofu ziona, bolemala mendo bayenda, bamakate bapola, ba chiulu bamvela futi, bakufa baukisiwa nafuti, na utenga ulalikiliwa kuli baja bosauka. ⁶ Odalisika niuja wamene sakalipa chifukwa cha ine." ⁷ Pamene aba bantu banali kuyenda pa ntchito yabo, Yesu anayamba kuuza magulu pali Yohane kuti, "Nanga kansi mwenze munayenda kuona chani muchipululu-ka uzu konyangányisiwa na chipembo?" ⁸ Nanga nichani chamene mwenze mwayenda kuona kansi-muntu wamene avala vovala vabwino? Zoona, baja bamene bavala vovala vabwino bankala mu manyumba ya ufumu. ⁹ Kansi mwenze mwa enda kuona chani-muneneli? Zoona, nikuuzani imwe, koma futi kuchilapo napali muneneli chabe. ¹⁰ Uyu ndiye wamene vinelembewapo vokamba kuti, 'Ona, nizatuma wautenga wanga pamenso yanu, wamene azakukonzelani njila.' ¹¹ Nikamba kuli imwe chazoon, pali bonse wobadwa kuli bakazi kulibe mukulu ochila Yohane Mubatizi. Koma uja wochepa mu ulemelelo mu ufumu waku mwamba amuchila uyu. ¹² Kuyambila masiku ya Yohane Mubatizi kufikila apa mamnje, ufumu wakumwamba wavutika na pokoso, na baja bapokoso bautenga mwa mpavu. ¹³ Chifukwa bonse baneneli na malamulo yanali kunenela kufikila mpaka Yohane; ¹⁴ ngati ndimwe bokonzekela kuchivomela ichi, uyu ndiye Eliya wamene anali kubwela. ¹⁵ Wamene ali na matu yamene yamvela, mulekeni amvele. ¹⁶ Kansi uyu mubadwe ninga ulinganisane na chani? Uli monga bana bamene basobela pa malo yama londa, bamene bankala nakuitanana wina na munzake ¹⁷ naku kamba kuti, 'Takulinzila mutolilo iwe, koma iwe sunavine. Talila, koma iwe sunalileko.' ¹⁸ Chifukwa Yohane sanabwele akudya kapena na kumwa vinyu, koma bakamba kuti, 'ali na chibanda.' ¹⁹ Mwana wa Muntu anabwela akudya na kumwa bakamba kuti, 'Onani, nikamukonda kudya nafuti ni chakolwa, munzake waba musonko na bantu bamachimo!' Koma nzelu zima weluzika zolungama kulangana zna ntchito ake" ²⁰ Yesu anayamba kukalipila mizinda mwamene ntchito zake zikulu zinachitikiliwa, chifukwa sibama tembenuke. ²¹ "Soka kuli iwe, Kolazini! Soka kuli iwe, Betisaida! Chifukwa ngati nthito zamene zachitika mukati mwanu asembe zinachitikiliwa mu Tayala na mu Sidoni, asembe banatembenuka kudala bali vale na vovala vama saka na milota. ²² Koma chozabankalilako bwino baku Tayala na Sidoni pa siku ya chiweluzo kuchila imwe. ²³ Iwe, Kapenamu, uganiza monga uzakwezewa kumwamba? Iyayi, uzaponyewa mu Hadesi. Chifukwa ngati nthito zikulu zamane zachitiwa muli iwe asembe zinachitikiwa muli Sodoma, asembe nalelo ikaliko nalelo. ²⁴ Koma nikuuzani imwe kuti chizainkalilapo bwino ziko ya Sodoma pa siku ya chiweluzo kuchilapo imwe." ²⁵ Pa ntawi ija Yesu anakamba kuti, "Nikutamandani imwe, Atate, Ambuye wakumwamba na wa paziko lapansi, chifukwa munabisa ivi vintu kuli baja bantu banzeli na baja bomvesesa, koma mwavizibisa kuli bana bagóno. ²⁶ Zoona, Atate, chifukwa ichi chinali chinakumvesani bwino imwe. ²⁷ Vonse vintu vinapasiwa kuli ine kuchokela kuli ba Tate; futi kulibe wamene aziba Mwana koma chabe ba Tate, kulibe wamene aziba ba Tate koma chabe Mwana na muntu aliwonse wamene Mwana asanka kuti amuzibise. ²⁸ Bwelani kuli ine, bonse bamene mu sebenza mwalemesewa na katundu, ndipo nizakupasani kupumula. ²⁹ Tengani goli yanga pali imwe ndipo punzilani kuli ine, chifukwa ine ndine ozichepesa nafuti ozibwesa mutima, ndipo muzapeza kupula kwa moyo zanu. ³⁰ Chifukwa goli yanga siyovuta na katundu wanga niwopepuka."

Chapter 12

¹ Pa ntawi ija Yesu anali ku enda-enda mu munda wa tiligu pa siku ya Sabata. Bopunzila bake banamvela njala bana yamba ku tyola tiligu naku dya. ² Koma pamene ba Falisi banaona ichi, banauza Yesu kuti, "Ona, bopunzila bako bachita chintu chamene chipwanya lamulo ya pa Sabata." ³ Koma Yesu anabauza kuti, "Nanga munabelenga vamene Davide anachita pamene anamvela njala, pamozi na bamuna bamene anali nabo?" ⁴ Anaenda mu nyumba ya Mulungu nakudya buledi ya kupezekapo, chintu chamene sichinali chovomelesewa kuti adye na baja bamene banali pamozi na eve, koma chovomelesewa chabe kuli ba nsembe. ⁵ Nanga simunabelenge mu malamulo kuti pa Sabata ba nsembe mu nyumba ya Mulungu bama pwanya Sabata koma balibe chimo? ⁶ Koma niku uzani imwe kuti umozi mukulu ochila tempele alipo pamalo pano. ⁷ Asembe munaziba chamene ichi chitantaufa, 'Ine nifuna chifundo osati nsembe,' asembe simuna weluze muntu alibe chimo. ⁸ Chifukwa Mwana wa Muntu ni Mfumu ya Sabata." ⁹ Pamene apo Yesu anachokapo naku yenda mu Sinagogo yabo. ¹⁰ Onani, munali muntu wamene anali na kwanja yoyuma. Ba Falisi banamufunsa Yesu, kuti, "Nanga nichovomelesewa kupolesa bantu pa Sabata?" kuti bamunamizile kuti achimwa. ¹¹ Yesu anakamba kuli beve kuti, "Nanga ni muntu uti pakati panu, wamene, ngati anali na nkosa imozi chabe, yamene iyi nkosa yabwela yagwela mu mugodi ukulu pa Sabata, sazai gwila nakuichosamo?" ¹² Nanga nikuchilapo kwa bwanji, kansi, umoyo wa muntu pa wa nkosa! Chifukwa chake nichovomelesewa kuchita chintu chabwino pa Sabata." ¹³ Pamene apo Yesu anakamba kuli uja mwamuna kuti, "Tembenula kwanja yako." Anaitembenula kwanja, inabwezewa kunkala ya tanzi, monga ija kwanja inangu. ¹⁴ Koma ba Falisi bana enda naku yamba ku lingilila malingo pa umoyo wake. Banali kusakila njila yamene wanga mupaille. ¹⁵ Pamene Yesu anaziba ivi, anachokako kumalo kuja. Bantu bambili banamukonka, ndipo anabachilisa bonse. ¹⁶ Anabauza kuti basazibise bantu bali bonse pali eve, ¹⁷ kuti chinkale cha zooni, chamene chinakambiwa kupitila muli muneneli Yesaya, kukamba kuti, ¹⁸ "Onani, wantchito wanga wamene ninasanka; okondewa wanga, wamene moyo wanga umvela bwino. Nizaika Muzimu wnga pali eve, azalalikila chiweluzo kuli bakunja. ¹⁹ Eve sazavutana kapena kupunda; kulibe wamene azamvela liu yake munjila. ²⁰ Sazatyola ntete yo onongeka; saza zimya nyali yamene ichosa chusi, kufikila pamene eve azasogolela kupambana, ²¹ na muzina yake ba Kunja bazapezamo chiyembekezo." ²² Umozi mpofu wamene anali chi ulu nafuti, wamene anali na chibanda, banamuleta kuli Yesu. Anamupolesa, kulengesa kuti uja muntu ayambe kuona naku kamba. ²³ Magulu yonse yanadabwa nakukamba kuti, "Nanga uyu mwamuna kansi angankale ndiye Mwana wa Davide?" ²⁴ Koma ba Falisi pamene banamvela va vodabwisa ivi, banakamba kuti, "Uyu muntu samachosa chabe vibanda asebenzesa Biluzibabu, mukulu wa vibanda." ²⁵ Koma Yesu anaziba maganizo yabo naku bauza kuti, "Ufumu uli onse wamene ugabika paweka uonongeka, na muzinda uli onse kapena nyumba yamene igabikana payeka siizaimilila. ²⁶ Ngata Satana achosa Satana, agabikana eka kansi. Nanga ufumu wake uzaimilila bwanji?" ²⁷ Ngati ine nichosa vibanda kusebenzesa Belizababu, nanga bana banu basebenzesa chani? Chifukwa cha ichi nkalani boziweluzani mweka. ²⁸ Koma ngati ine nichosa vibanda kusebenzesa Muzimu wa Mulungu, ufumu wa Mulungu wabwela kuli imwe. ²⁹ Nanga muntu angangene bwanji mu nyumba ya muntu wampavu nakumubela vintu osayambilila kumangilila muntu wampavu? Akachita ichi anga kwanise nakuba vintu vake va munyumba. ³⁰ Uja wamene sali naine ashushana naine, nauja wamene sakololela pamozi naine ndiye wamene ataya. ³¹ Chifukwa chake nikuuzani kuti, chimo ili yonse naku nyozela kuli konse muzakululukiliwa, koma kunyozela Muzimu sikuzakululukiliwa. ³² Ali onse wamene akamba mau yonyoza Mwana wa Muntu, azakululukiliwa. Koma uja wamene anyozela Muzimu Oyela, uja sazakululukiliwa, muziko ino, kapena muziko yamene izabwela. ³³ Lengani mutengo unkale wabwino na vipaso vake vizankala wabwino, chifukwa mutengo umazibika na vipaso vake. ³⁴ Imwe bana banjoka, chifukwa ndimwe boipa, nanga mungakambe bwanji vintu wabwino? Chifukwa kuchokela mu kuzula kwa vintu wamene vili mu mutima ndiye wamene kamwa kakamba. ³⁵ Uja muntu wabwino kuchokela mu tumba yake yaku mutima yabwino amachosa vintu wabwino, na uja muntu oipa kuchokela mu tumba yake yaku mutima yoipa achosa voipa. ³⁶ Niku uzani kuti pa siku yoweluza bantu bazakaweluziwa pa mau yali yonse yamene yalibe pindu yamene bakamba. ³⁷ Chifukwa ni mu mau yako mwamene iwe uzaonesa kulangama, na mu mau ndiye mwamene uzaweluziliwa." ³⁸ Pamene apo bena bolemba na ba Falisi banamuyanka Yesu kuti, "Mupunzisi, ise tifuna kuona choonesi kuli iwe." ³⁹ Koma Yesu anabayanka kuti, "Mubadwe oipa wachigololo ufuna cho-onesela. Koma kulibe cho-onesela chamene chizapasiwa koma chabe cho-onesela cha Yona muneneli. ⁴⁰ Monga mwamene Yona analili ma siku yatatu na mazuba yatatu mu mala mwa chinsomba chikulu, chimozi-mozi mwamene Mwana wa Muntu azankalila masiku yatatu na mazuba yatatu mu mutima wa ziko. ⁴¹ Bantu baku Nineve bazakaimilila pa siku yoweluza pamozi na mubadwe uyu naku iweluza. Chifukwa beve banatembenuka chifukwa cha kulalikila kwa Yona, koma onani, mukulu ochila na pali Yona ali po pano. ⁴² Mfumu mukazi wakumwela azakaimilila pa siku yoweluza pamozi na bantu ba mubadwe uno naku

baweluza. Eve anabwela kuchokela kosilizila ziko kuti akamvele nzelu za Solomoni, koma onani, muntu mukulu pali Solomoni ali pano. ⁴³ Pamene muzimu wadoti uchoka mumuntu, uma pita mu malo yamene yalibe manzi kusakila popumulila, koma siu upeza. ⁴⁴ Pamene apo ukamba kuti, 'Nizabwelela ku nyumba yanga kwamene ine ninachokela.' Pamene ubwelela, upeza kuti nyumba ija niyopyangiwa na vintu voikiwa mumalo mwake. ⁴⁵ Umabwela waenda kukatenga kubwela nazo mizimu zinangu zili seveni zamene zinkala zoipisisa kuchila yeve, babwela naku nkala mukati mwake muntu uyu. Posilizila pake nipakuti uja muntu azankala ochilapo kulinganisana na poyamba. Nimwa mene chizankalila na uyu mubadwe oipa." ⁴⁶ Pamene Yesu anali akali kukamba na gulu ya bantu, onani, ba mai bake na babale bake banaimilila panja, kufuna kuti bakambe na eve. ⁴⁷ Umozi pali eve anakamba kuli eve kuti, "Onani, bamai bako na babale bako bali imilile panja, bafuna kukamba naiwe." ⁴⁸ Koma Yesu anayanka nakukamba kuli eve kuti, "Nanga nindani mai wanga kapena nibati ba bale banga?" ⁴⁹ Pamene apo anatambasula kwanja yake kulangiza kunali bopunzila bake nakukamba kuti, "Onani, aba bali apa ba mai banga na babale banga! ⁵⁰ Chifukwa muntu ali onse wamene achita chifunilo cha ba Tate banga bamene bali kumwamba, uja muntu ndiye mubale wanga, mulongo wanga, mai wanga."

Chapter 13

¹ Pa siku yamene ija Yesu ana enda panja pa nyumba naku nkala pambali pa nyanja. ² Gulu ikulu ina unjikana kumuzungulukila, pamene apo anangena mu bwato naku nkala mwamene muja pamene gulu yonse inaimilila posilizila nyanja. ³ Yesu anakamba nabo vintu vambili kupitila mu myambo. Anakamba kuti, "Onani, mulimi anaenda kuka shanga mbeu. ⁴ Pamene anali kushanga, mbeu zinangu zinagwela mumbali mwa museu, tunyoni tunabwela twaizidya. ⁵ Zinangu mbeu zinagwela pa myala, pamene zinalibe ntaka yambili. Pamene apo zinamela chifukwa ntaka siinali yongena pansi maningi. ⁶ Koma pamene zuba inaima, zina ochewa chifukwa zinalibe mizyu, ndipo zinayuma. ⁷ Mbeu zinangu zinagwela pakati pa minga. Minga zinamela naku kama mbeu izi. ⁸ Zinangu mbeu zinagwela pa ntaka yabwino zinamela naku nkala na vipaso vabwino, zinangu makumi yali kumi kuchilapo, zinangu makumi asanu na imozi, ndipo na yenangu makumi yatatu. ⁹ Wamene ali na matu, mulekeni amvele." ¹⁰ Bopunzila banabwela kuli Yesu nakukamba kuti, "Nanga nichani mukamba nagulu mu myambo?" ¹¹ Yesu anaba yanka kuti, "Imw munali nao mwai womvesesa vobisika va mu ufumu waku mwamba, koma kuli beve sichina pasiwe ichi. ¹² Chifukwa kuli wamene ali navo vambili vizapasiwa, ndipo azankala navambili. Koma kuli uja wamene alibe, na vamene ali navo vizapokewa. ¹³ Ichi ndiye chifukwa chake chamene nibauzila kupitila mu miyambo: ngakale kuti babelenga, koma sibaona; bangankale bamvela, koma sibamvesesa. ¹⁴ Kuli beve uneneli wa Yesaya ufikilisiwa, wamene unakamba kuti, 'Ngakale kuti kumvela muzayamba kumvela, koma kulibe njila yamene muzamveseselamo; ngakale kuti muona, koma kulibe njila yamene munaonelamo. ¹⁵ Chifukwa mitima za aba bantu zinankala zosamvela, sibamvela naku mvela, ndipo bana vala na menso yabo, kuti basakwanise kuona na menso yabo, kapena kumvel na matu yabo, kapena kumvesesesa na mitima zabo, kuti batem enuke, kuti ine niba polese.' ¹⁶ Koma menso yanu niyodalisisika, chifukwa yaona; na matu yanu, chifukwa ya mvela. ¹⁷ Zoonu nikuuzani imwe kuti bambili baneneli na bantu bolungama banali kufunisika kuti baone vintu vamene imwe muona koma sibana vione. Banafunisika kuti bamvele vintu vamene imwe mumvela kuma sibana vimvele. ¹⁸ Mvesesani kuli ntano ya mulimi wamene ana shanga mbeu zake. ¹⁹ Pamene muntu ali onse amvela mau ya ufumu koma samvesesa tautauzo yake, uja oipa amabwela naku jompola chamene chashangiwa mumutima wake. Iyindiye mbeu yamene inali inashangiwa mumbali mwa museu. ²⁰ Chamene chinashangiwa pa myala ni uja muntu wamene amamvela mau na pamene apo amayalandila mokondwela, ²¹ koma alibe mizyu muli eve ama limbikila pangóno chabe. Pamene mavuto kapena kuvutikisiwa kubwela chifukwa cha mau, akugwa kamusanga. ²² Chamene chinashangiwa pakati pa minga, ndiye uja muntu wamene amamvela mau, koma kukonda va muziko na boza ya chuma vima kama mau aya, ndipo ankala alibe vipaso. ²³ Mbeu yamene imashangiwa pa ntaka ya bwino, niuja muntu wamene amamvela mau naku yamvesesa. Ama nkala na vipaso, kubala mumozi handeledi, mwinangu sikiste, na mwinangu ma sate kupitililapo pali vamene anashanga." ²⁴ Yesu anabapasa myambo ina. Anakamba kuti, "Ufumu wa kumwamba uli monga muntu wamene anashanga mbeu yabwino mu munda wake. ²⁵ Koma pamene anali gone, mudani wake anabwela naku shanga mau uzu pakati pa tiligu naku yenda. ²⁶ Pamene matepo yanamela naku nkala na vipaso vabo, na mauzu yanaonekela na yeve. ²⁷ Ba ntchito ba uja mwine wa munda anabwela nakukamba kuli eve kuti, 'Bwana, nanga kansi siti nashange mbeu yabino yeka chabe? Nanga nichani mwamela mau uzu?' ²⁸ Anaba yanka kuti, 'Mudani ndiye wamene achita ivi.' 'Bantchito bana kamba kuti, 'Nanga mungativomeleze kuti tiyende tikanyule mau uzu?' ²⁹ 'Mwine wa munda anayanka kuti, 'Iyayi. Chifukwa pamene imwe muzayamba kunyula mau uzu, munganyulile pamozi na tiligu. ³⁰ Vilekeni vimelele pamozi chabe. Pa ntawi yokolola nizakabauza bokolola kuti, 'Yambililani kuchosa ma uzu muyamangilile nakuyamangilila muya oche naku yaocha, koma tiligu yeve muyi kolole mui ike mu chibaya changa.' ³¹ Yesu anabauza mwambo winangu beve. Anakamba kuti, "Ufumu waku mwamba uli monga ka mbeu kampiru kamene muntu anatenga naku shanga mu munda wake. ³² Aka kambeu nika ngóno pa mbeu zonse. Koma kaka kula, ndiye kankala kakulu pali vomela vonse mumunda. Chimankala chimutengo, mwakuti tu nyoni twa kumwamba tumabwela naku pumulila muli cheve." ³³ Yesu pamene apa anabauza mwambo wina. "Ufumu waku mwamba uli monga chotupisa chamene muzimai anatenga naku ika mu vigawa vitatu va fulawa kufikila mpaka fulawa ija inatukumuka." ³⁴ Vonse ivi vintu Yesu anali ku uza magulu kupitila mu myambo; sanali kukamba na babo bantu bantu ngati sanasebenzese myambo. ³⁵ Chifukwa chake chinali chakuti vintu vamene vina kambiwa na muneneli vikachitike, pamene anakamba kuti, "Niza segula kamwa kanga mu myambo. Niakamba vintu vamene vinali vobisika kuchokela koyambila kwa ziko." ³⁶ Pamene apo Yesu anayasiya magulu naku enda munyumba. Bopunzila bake banabwela kuli eve nakukamba kuti, "Tiuzeni tautauzo ya myambo ya ma uzu mu munda." ³⁷ Yesu anabayanka nakukamba kuti, "Uja wamene ashanga mbeu ni Mwana wa Muntu. ³⁸ Munda ni ziko; ija mbeu yabwino, ndiye baja bana bamu ufumu. Mau uzu ndiye bana ba mudani, ³⁹ mudani wamene anashanga mbeu zija ni mudani. Kukolola ndiye kusila kwa mubadwe,

bokolola ni bangelo. ⁴⁰ Chifukwa chake, monga mwamene mauzu bamaya chosela naku yashoka na mulilo, ndiye mwamene chizankalila paku sila kwa mubadwe. ⁴¹ Mwana wa Muntu azaka tuma bangeli bake, bazaka ika pamozi kuchosa mu ufumu wake vintu vonse vamene vima lengesa kuchimwa nabaja bamene bachita machimo. ⁴² Bazaba taya mumuli, mwamene muzankala kulila naku sheta meno. ⁴³ Pamene apo baja bolungama bazaka unikila monga zuba mu ufumu waba Tate wabo. Wamene ali na matu, mulekeni amvele. ⁴⁴ "Ufumu wa kumwamba uli monga chuma chamene chinavisiwa mu munda. Muntu anachipeza nakuchibisa. Mukukondwela kwake aenda, nakugulisa vintu vake vonse vamene alinavo, naku gula uja munda. ⁴⁵ Chimozi-mozi, ufumu wa kumwamba uli monga muntu wamalonda wamene asakila sakila myala zamutengo wapatali. ⁴⁶ Pamene anapeza mwala umozi wamutengo wapatali, anaenda naku gulia vonse vamene anali navo naku ugula. ⁴⁷ "Futi, ufumu waku mwamba uli monga chokokela nsomba chamene chinaponyewa mu nyanja, chamene china gwila vintu vosiya siyana. ⁴⁸ Pamene china zula, bogwila nsomba banachi donsa kuchileta kumbali kwa manzi. Bana nkala pansi naku tengamo vija vabwino kuvi ika muma lubango, koma vija vamene vinalibe ntchito banavitaya. ⁴⁹ Chizakankala chimozi-mozi pa kusila kwa mubadwe. Bangeli bazakabwela naku patulisa baja boipa kobachosa kuli baja bolungama. ⁵⁰ Bazabataya mumulilo, mwamene muzankala kulila naku sheta meno. ⁵¹ "Nanga mwamvesesa ivi vintu mwati?" Bopunzila bake banamuyanka naku kamba kuti, "Eeeh." ⁵² Pamene apo Yesu anabauza kuti, "Chifukwa cha ichi ali onse kalembela wamene ankala opunzila mu ufumu waku mwamba ali monga muntu wamene ndiye mwine wa nyumba, wamene achosa vintu vonse vasopano navija vakudala kuchosa mosungila mwake." ⁵³ Pamene Yesu anasiliza izi myambo, anachokako kuja kumalo. ⁵⁴ Yesu anabwelela kumalo kwake naku yamba kupunzisa bantu muma Sinagogo yabo. Pindu yake inali yakuti banali bodabwa kwambili naku kamba kuti, "Kansi uyu muntu izi nzelu azichosa kuti na ivi vodabwisa?" ⁵⁵ Nanga uyu siwamene mwana wa mupala ma tabwa? Nanga mai wake siuja Maria? Nanga wabale bake sibaja bene Yakobo, Yosefe, Simoni, na Yudas? ⁵⁶ Nanga balongo bake sitinkala nabo kansi? Nanga ivi vintu vonse kansi anavichosa kuti?" ⁵⁷ Banakalipa naye. Koma Yesu anabauza kuti, "Muneneli amalandila ulemu kuli konse kuchoselako chabe mu ziko yake na ku banja yake." ⁵⁸ Sanachite vodabwisa vambili kuja chifukwa cha kukana kukulupilila kwabo.

Chapter 14

¹ Pantawi ija, Helodi umozi mwa basogoleli anamvela uthenga wa Yesu. ² Anauza bantchito bake kuti, "Uyu niwamene Yogane Obatiza; auka kubakufa. Ndiye chamene chilengesa mpavu kusebenza muli eve." ³ Chifukwa Helodi anamugwila Yohane, nakumumanga, nakumuika mu ndende chifukwa cha Helodiyasi, mukazi wa Filipu mubale wake. Chifukwa ⁴ Yohane anamuza kuti, "Sichintu chovomelesewa kuti uyu ankale mukazi wako." ⁵ Helodi anafuna kumupaya, koma anali kuyopa bantu, chifukwa banali kumuyopa kukamba kuti nimuneneli. ⁶ Koma siku yokumbukila kubadwa kwa Helodi inafika, mwana mukazi wa Helodiyasi anavina pakati pa bantu nakumvesa bwino Helodi. ⁷ Pakuona ichi, anamulonjeza lonjezo molapa kuti azamupasa chintu chili chonse chamene azapempa. ⁸ Pamene bamai bake banamuza vopempa, anakamba kuti, "Nipaseni apa manje, pa mbale, mutu mwa Yohani Obatiza." ⁹ Mfumu inakalipa maningi chifukwa cha chamene anapempa, manje chifukwa chakuti analapa na chifukwa cha baja bantu bamene banali naye pa chakudya chaku mazulo, anakamba kuti ichi chamene chichitike. ¹⁰ Anatomiza kuti bayende bamupaye Yohane mu ndende. ¹¹ Ndipo mutu wake unabwelesewa pa mbale naku pasiwa kuli mwana mukazi uja wamene anautenga naku upeleka kuli bamai bake. ¹² Bopunzila bake banabwela, nakunyamula thupi yake, naku yenda kuiika mumanda. Kuchoka apa, banayenda kukamuza Yesu. ¹³ Manje pamene Yesu anamvela ichi, anachokako uku naku enda ku malo kwa eka. Pamene magulu yanamvela ichi, banamukonnka Yesu na mendo kuchokela mu mizinda. ¹⁴ Yesu anabwela kwamene kunali beve nakuona gulu ikulu maningi. Anamvela chifundo nakubapolesela bantu bodwala babo. ¹⁵ Ntawi yaku mazulo, bopunzila banabwela kuli eve nakumuza kuti, "Kuno kumalo kulibe bantu, na ntawi yasila. Balekeni bantu, basiyeni bayende mu minzi kuti bakagule vakudya badye." ¹⁶ Koma Yesu anabayanka kuti, "Aba sibafunika kuti baende iyayi. Imwe mubapase vakudya." ¹⁷ Koma banamuyanka kuti, "Onani tili chabe na buledi ili 5 na nsomba zibili." ¹⁸ Yesu anayanka kuti, "Letani kuli ine." ¹⁹ Yesu anauza gulu kuti inkale pansu pa mauzu. Anatenga ma buledi yaja na nsomba zibili. Analangana kumwamba, anayadalisa ma buledi nakuya suna naku pasa bopinzila bake, na bopunzila bake banapasa ija gulu ya bantu. ²⁰ Bonse banadya naku kuta. Banatenga vamene vinasalapo - votengelamo vili kumi na vibili. ²¹ Baja bamene banadya banali 5000 bamuna, kochoselako bakazi na bana. ²² Pamene apo anauza bopunzila bake kuti bangene mu bwato bayende kumbali kwina kwa nyanja, pamene eve anali kupisha bantu. ²³ Pamene anasiliza kupisha bantu, anayenda pa chulu eka nakupempela. Pamene usiku unabwela, analipo eve eka. ²⁴ Koma bwato inali kutali pakati pa manzi, inali kugwedezeke na chimpepo, chifukwa chimpepo chinali chikulu. ²⁵ Mbanda kucha Yesu anafika kufupi na beve, nishi ayenda pa manzi. ²⁶ Pamene bopunzila bake banamuona ayenda pa manzi, banavutika mutima nakukamba kuti, "Nichibanda," banalila na manta. ²⁷ Koma Yesu anabauza pamene apo kuti, "Nkalani bolimba! Ndine! Osayopa iyayi." ²⁸ Petulo anamuyanka nakukamba kuti, "Ambuye, ngati ndimwe, niuzeni kuti ine nibwele pa manzi." ²⁹ Yesu anakamba kuti, "Bwela." Pamene apo Petulo anachoka mu bwato naku yenda pa manzi kuyenda kuli Yesu. ³⁰ Koma pamene Petulo anaona chimpepo, anayopa, pamene anayamba kumbila, analila nakukamba kuti, "Ambuye, nipulumuseni!" ³¹ Yesu pamene apo anatambasula kwanja yake, nakumugwila Petulo, nakumuza kuti, "Iwe wachikululupilo chingono, nanga nichani chamene wenze wakaikilila?" ³² Manje pamene Yesu na Petulo banangena mu bwato, chimpepo chija chinaleka. ³³ Baja bopunzila bake bamene banali mu bwato banamupembeza Yesu naku kamba kuti, "Zooni ndimwe Mwana wa Mulungu." ³⁴ Pamene beve banafika kumbali kwingu kwa nyanja ija, banafikila kumalo yaku Genezaleti. ³⁵ Pamene bantu bakuja kumalo banamuziba Yesu, bana tuma mau monse mu malo ya mumbali, ndipo banaleta bantu bonse bodwala. ³⁶ Banamupapatila kuti bagwileko chabe chovala chake, ndipo bonse bamene banamugwila banapolesewa.

Chapter 15

¹ Ba Falisi naba Bolemba banabwela kuli Yesu kuchokela ku Yelusalemu. Banakamba kuti, ² "Nanga nichani bopunzila bako sibakonka myambo za makolo? Chifukwa sibasamba kumanja pakudya." ³ Anabayanka kuti, "Nanga naimwe nichani chamene mupwanyila lamulo ya Mulungu chifukwa cha myambo zanu?" ⁴ Chifukwa Mulungu anakamba kuti, 'Lemekeza batate bako na bamai bak', nafuti kuti 'Eve wamene anyoza ba tate bake kapena bamai bake azapaiwa.' ⁵ Koma imwe mukamba kuti, 'Ali onse wamene auza tate wake kapena mai wake kuti, "Tandizo ili yonse yamene imwe munalandila kochokela kuli ine ni mpaso yopelekewa kuli Mulungu," ⁶ wamene uja muntu futi safunikila kulemekeza batate bake.' Chifukwa cha ichi mwalengesa kuti mau ya Mulungu yankala yalibe mpavu chifukwa cha myambo zanu. ⁷ Imwe bantu baboza! Zoonza mwamene Yesaya ananenela pali imwe pamene anakamba kuti, ⁸ 'Aba bantu banilemekeza chabe pakamwa, koma mitima zabo zili kutali na ine.' ⁹ Bapembeza ine mwachabe chifukwa bapunzisa kunkala vipunziso malamulo ya bantu." ¹⁰ Anabwela aitana gulu kuti ibwele kuli eve naku iuza kuti, "Mvelani nafuti mumvesese- ¹¹ Kulibe chintu chamene chingena mukamwa naku lakwisa muntu uyo. Koma, chamene chichoka mukamwa, ndiye chamene chima lakwisa muntu. ¹² Bopunzila banabwela naku mu-uza Yesu kuti, "Nanga muziba kuti ba Falisi bamakalipa bakamvela mau aya?" ¹³ Yesu anabayanka nakukamba kuti, "Mutengo uli onse wamene ba Tate banga sibana shange uzanyuliwa." ¹⁴ Basiyeni beka, nibasogoleli balibe menso. Ngati mpofu asogolela mpofu winangu, bonse bazagwela mumugodi." ¹⁵ Yesu anayanka nakukamba kuti, "Tiuzeni chikambidwe ichi." ¹⁶ Yesu anayanka kuti, "Naimwe monse simuziba kukamba uku?" ¹⁷ Nanga simumaona kuti chintu chilichonse chamene chingena mukamwa chima enda mumala naku choka kuyenda muchimbuzi? ¹⁸ Koma vintu vamene vamachoka mukamwa vimachokela mumutima. Ivi ndiye vintu vamene viononga muntu. ¹⁹ Chifukwa mumutima wa muntu ndiye mwamene mumachokela maganizo yoipa, kupaya, vigololo, uchiwelewele, ukawalala, ukamboni waboza, na kunyozela. ²⁰ Ivi ndiye vintu vamene vima ononga muntu. Koma kudya pamene sunasambe kumanja sikumaononga muntu. ²¹ Pamene apo Yesu anenda kuchoka kuja kumalo naku yenda kumalo yaku dela yaku Taya naku Sidoni. ²² Onani, muzimai waku Kanani anabwela kuohekela kumalo yaja. Anapunda naku kamba kuti, "Nimvelelenikoni chifundo ine, Ambuye, Mwana wa Davide! Mwana wanga mukazi atengewa maningi nachibanda." ²³ Koma Yesu sanamuyanike mau yali yonse muzimai uyu. Bopunzila bake banabwela nakumupapatila kukamba kuti, "Mupisheni uyu aende, chifukwa atipundila ise." ²⁴ Koma Yesu anayanka naku kamba kuti, "Ine sininatumiwe ku muntu ali onse koma chabe kuli nkosa za munyumba ya Izilayeli." ²⁵ Koma anabwela naku gwada pamenso pake, nakukamba kuti, 'Ambuye, nitandizeni ine.' ²⁶ Anamuyanika naku kamba kuti, "Sichintu chabwino kutenga buledi yabana naku itaila kuli tu imbwa tubana." ²⁷ Anakamba kuti, "Zo-ona, Ambuye, koma na tu imbwa tung'ono tumadya votaikila kuchoka podyela bene bake." ²⁸ Pamene apo Yesu anayanka nakumuza eve kuti, "Muzimai, uli na chikulupililo chikulu; leka chikuchitikile monga mwamene iwe ufunila." Pamene apo mwana wake mukazi uja anapola. ²⁹ Yesu anachokako kumalo kuja naku yenda ku nyanja yaku Galilea. Anaenda akwela pa lupili naku nkala pamene paja. ³⁰ Magulu yabantu yanamukonka. Banamuletela bantu bolemala, mpofu, bachi ulu, na bantu bopunduka, na baja bamene banali bodwala. Banabaika pafupi na Yesu, anabapolesa. ³¹ Gulu ija inadabwa kwambili pamene banaona bachi ulu bayamba kukamba, bopunduka bapola, bolemala bayenda, na mpofu ziona. Banatamanda Mulungu waku Izilayeli. ³² Yesu anaitana bopunzila bake nakubauza kuti, "ine gulu ya bantu yanimvesa chifundo chifukwa chakuti bankala naine masiku yatatu pamene apa koma balibe na vakudya. Sinifuna kuba pisha bakalibe kudya kali konse, chifukwa banga komoke munjila." ³³ Bopunzila banamuza kuti, "Manje nanga nikuti kwamene tingagule mukate wamene ungakwanile kudyesa gulu ikulu iyi ya bantu kuno kumalo kwamene sikunkala na bantu?" ³⁴ Yesu anabayanka kuti, "Nanga ma buledi yamene muli nayo niya ngati? Bana yanka kuti, "Yali seveni, na tu nsomba tung'ono." ³⁵ Yesu anabauza gulu ija kuti inkale pansi." ³⁶ Anatenga ma buledi yali seven yaja na nsomba, pamene ana yamika, ana suna ma buledi yaja naku yapasa kuli bopunzila bake. Bopunzila bake bana gabisa gulu. ³⁷ Bantu bonse banadya naku kuta. Bana tenga ma buledi yanasalako muma basketi. ³⁸ Baja bamene banadya banali four sauzande bamuna, kosapendelako bazikazi na bana. ³⁹ Kuchoka apa Yesu anapisha yaja magulu kuti yayende pamene apo anakwela mu bwao naku yenda ku malo yaku Magadana.

Chapter 16

¹ Ba Falisi naba Saduki banabwela kumuyesa eve kumufunsa kuti abalangise cholangiza chokokela kumwamba. ² Koma anabayanka nakubauza kuti, "Pamene ikali ntawi yaku mazulo, mumakamba kuti, 'Kuzankala bwino lelo, chifukwa makumbi yaoneka monga ma magari.'" ³ Pamene kukucha, mumakamba kuti, 'lelo kzankala mpepo, chifukwa makumbi yaoneka monga magari nafuti yavala kumwamba.' Imwe muziba tantauzo ya kaonekedwe ka makumbi, koma mukangiwa kuziba voonesha ntawi. ⁴ Mubadwe woipa wa chigololo ifunisisa choonesha, koma kulibe choonesha chamene chizapasiwa koma cha Yonah cheka." Pamene apo Yesu anabasiya naku enda. ⁵ Pamene bopunzila banafika kumbali ina, banaibala kunyamula buledi. ⁶ Yesu anabauza kuti, "Nkalani bochenjela ku votupisa vaba Falisi na ba Saduki." ⁷ Bopunzila banayamba kukambisana pakati pabo kuti, "Nichifukwa chakuti sitinanyamule buledi." ⁸ Yesu anaziba kuganiza kwabo nakubauza kuti, "Imwe ba chikulupililo chingóno, nanga nichani mukambisana pamweka kuti nichifukwa chakuti simunanyamule buledi?" ⁹ Nishi simuona kapena kukumbuka ma buledi yaja yanali 5 ya bantu banali 5000, na mabasiketi yamene munatengelamo vinasala? ¹⁰ Kapena ma buledi yanali 7 ya bantu banali 4000, na mabasiketi yamene yanasalapo yamene munatenga? ¹¹ Nanga nibwanji imwe simuona kuti sininali kukamba naimwe pali buledi? Nkalani wochenjela na votupisa vaba Falisi naba Saduki." ¹² Pamene apa banaziba kuti sanali kubauza kuti basachenjele chifukwa cha chotupisa cha buledi, koma kuti bankale wochenjela chifukwa cha vipunziso vaba Falisi naba Saduki. ¹³ Pamene Yesu anabwela kumalo pafupi na Sizaliya na Filipi, anabafunsa bopunzila bake kuti, "Nanga bantu kansi bakamba kuti Mwana wa Muntu nindani?" ¹⁴ Banamuyanka kuti, "Benangu bakamba kuti ndiwe Yohane Mubatizi; benangu bakamba kuti Eliya; na benangu, Yelemiya, kapena umozi opunzila wa baneneli." ¹⁵ Anabauza kuti, "Nanga imwe mukamba ine ndine ndani?" ¹⁶ Mukuyanka, Simoni Petulo anakamba kuti, "Ndimwe Kristu, Mwana wa Mulungu wa moyo." ¹⁷ Yesu anayanka naku muuza kuti, "Ndiwe odalisika, Simoni mwana wa Yonah, chifukwa tupi na magari sivamene vakuzibisa ichi, koma ba Tate banga bamene bali kumwamba. ¹⁸ Nikuuzza futi kuti iwe ndiwe Petulo, pa mwala wamene uyu ine nizamanga kachisi yanga. Viseko vaku Hadesi sivizakwanisa kupambana. ¹⁹ Nizakupasa mfungulo yaku ufumu wa kumwamba. Chilichonse chamene uzamanga pa ziko ya pansi chizamangiwa kuziko yaku mwamba, na chili chonse chamene uzamangusula paziko yapansi chimangusuliwa kumwamba." ²⁰ Yesu anauza bopunzila bake kuti basauzeke muntu aliwonse kuti eve ni Kristu. ²¹ Kochokela ntawi yamene iyo Yesu anayamba kuuza wopunzila bake kuti eve afunika kuyenda ku Yelusalemu, akavutikisiwe mu vintu vambili mumanja yaba kulubakulu na bakulu ba nsembe na bolembe, akapaiwe, koma akauke kubakufa pa siku ya chitatu. ²² Petulo anamutenga kumbali Yesu naku mukalipila, kukamba kuti, "Ichi chinkale kutali naimwe, Ambuye; osati ivi vikakuchitikileni imwe." ²³ Koma Yesu anapindamuka nakuuza Petulo kuti, "Yenda kumbuyo kwanga ine, Satana! Ndiwe chogwesa ine, chifukwa susamalila vintu va Mulungu, koma chabe va bantu." ²⁴ Yesu anakamba kuli bopunzila bake kuti, "Ngati muntu aliwonse afuna kunikonka ine, ayenela kuzikana eka, anyamule mutanda wake, anikonke. ²⁵ Chifukwa aliwonse wamene afuna kupulumusa moyo wake azautaya, na uja wamene ataya moyo wake chifukwa cha ine azaupeza. ²⁶ Nanga pindu ilipati ngati muntu atenga ziko yonse koma ataya moyo wake? Nichichani chamene muntu angapase kuchinjanisa na moyo wake? ²⁷ Chifukwa Mwana wa Muntu azakabwela mu ulemelelo waba Tate bake pamozi nabangelo bake. Kuchoka apa azakapasa muntu aliwonse malipilo kulingana navamene anachita. ²⁸ Zoona nikuuzani imwe, pali benangu bamene bali imilile pano bamene sibazakaona imfa mpaka bakaone Mwana wa Muntu mu ufumu wake."

Chapter 17

¹ Ma siku yokumana yali sikisi Yesu anatenga Petulo, Yakobo, na Yohane mubale wake, nakukwela nabo pamwamba pa lupili pa beka. ² Anachinjisiwa pamenso pabo. Pa menso pake pabala monga zuba, na vovala vake vinankala vobala monga nyali. ³ Onani, banaonekela kuli beve Mose na Eliya ndishi bakamba na eve. ⁴ Petulo anavula kamwa nakukamkba kuli Yesu kuti, "Ambuye, nichabwino kuti ise kupeza pano. Ngati mufuna, nizapanga pano tu mitenge tutatu-kamozi kani, kamozi ka Mose na kenangu ka Eliya." ⁵ Pamene eve anali kukamba, onani, kumbi inaba vundikila, ndipo onani, munachoka mau mu kumbi, yokamba kuti, "Uyu ndiye Mwana wanga Wokondewa, wamene ine nimvela bwino. Mumveleleni." ⁶ Pamene bopunzila banamvela ivi, banagwada pansi namanta. ⁷ Yesu anabwela abagwila na kwanja nakukamba kuti, "Imani musachita manta." ⁸ Pamene apo banalanga kumwamba koma sibanaone ali onse koma Yesu eka chabe. ⁹ Pamene banali kubwelela kuchoka pa lupili, Yesu anabauza, kuti, "Musa uzeko muntu ai onse pali ivi vamene mwaona koma pamene Mwana wa Muntu azaka ukishiwa ku bakufa." ¹⁰ Bopunzila bake banamufunsa, kuti, "Nanga nichani bolemba bama kamba kuti Eliya ndiye wamene ayenela kuyambilila kubwela?" ¹¹ Yesu anabayanka nakukamba kuti, "Eeeh Eliyah ndiye wamene azayambilila kubwela kukonza vintu vonse." ¹² Koma nikuuzani imwe kuti, Eliya anabwela kudala, koma sibanamuzibe. Koma, banamuchitila vonse vamene banali kufuna kuli eve. Chimozi-mozi, Mwana wa Muntu azakavutika mumanja yabo." ¹³ Pamene apo bopunzila bake banaziba kuti anali kuba uza pali Yohane Obatiza. ¹⁴ Pamene banabwela kumene kunali gulu yabantu, mwamuna umozi anabwela kuli eve, anagwada pansi, naku kamba kuti, ¹⁵ "Ambuye, chitlanikoni chifundo mwana wanga, chifukwa adwala makate ndipo amavutika maningi. Kambili amagwela pa mulilo penangu mumanzi." ¹⁶ Nenze namu leta kuli bopunzila banu, koma bakangiwa kumupolesa." ¹⁷ Yesu anamuyanka, "Bosakulupilila mubadwe oónongeka, kansi ninkale naimwe ntawi itali bwanji? Kansi ninkale ozigwila ntawi itali bwanji? Muleteni kuno kuli ine." ¹⁸ Yesu anachikalipila chiya chi muzimu, chinachoka nochoka muli eve chiya chimuzimu, na uja mwana anapola ntawi yamene ija. ¹⁹ Bopunzila banabwela kuli Yesu pa beka nakukamba kuti, "Nanga nichani chamene ise takangiwila kuchichosa?" ²⁰ Yesu anayanka kuti, "Chifukwa ndimwe bochepe chikulupililo. Niku-uzani kuti, ngati muli nacho chikulupililo olo chochepe monga ka mbeu kampilu, munga chi uze ichi chi lupili kuti, 'Choka apa uyende paja,' ndipo chizafendela, kuli chamene chizankala choshupa kuli imwe." Ma buku yenangu yakudala maningi yalibe ndime ya 21 ²¹ "Koma ivi va mutundu uyu sivima choka koma ngati mwazimana chakudya na pempelo." ²² Pamene bakanali mu muzinda wa Galileya, Yesu anauza bopunzila bake kuti, "Mwana wa Muntu aza pelekewa mumanja ya bantu, ²³ ndipo bazamupaya, koma pa siku ya chitatu azakaukishiwa kubakufa." Bopunzila bake banankala bokalipa. ²⁴ Pamene banafika mu muzinda wa Kapenamu, bantu baja bamene banali kutenga ndalama za mu tempele banabwela kuli Petrosi nakumuza kuti, "Nanga bapunzisi banu bamalipila musonko wamu tempele?" ²⁵ Anabayanka kuti, "eeeh." Pamene Petrosi anabwela munyumba, Yesu anamufunsa kuti, "Nanga iwe uganizapo bwanji, Simoni? Nanga nikuli bandani kwamene mfumu za pa ziko zima tengako musonko kapena volipilisa? Kuli bana babo kapena bantu benangu chabe?" ²⁶ "Kuli bantu benangu chabe," Petulo anabayanka. Kansi ndishi bana nibomasuka," Yesu anamuyanka. ²⁷ Koma kuti ise tisa lengese bantu bamusonko kuti bachimwe, enda ku nyanje, uponye musozo, utenge nsomba yamene izayambilila gwiliwa. Uivule kamwa, uzapezamo ndalama. Itege uyende ukapase bamusonko kulipilila iwe na ine."

Chapter 18

¹ Pantawi yamene ija bopunzila ba Yesu banabwela kuli eve naku mufunsa kuti, "Nanga nindani mukulu mu ufumu wa kumwamba?" ² Yesu pamene apo anaitana ka mwana kangóno, naku kaika pakati pabo, ³ nakukamba kuti, "Zooni ni kuuzani imwe, ngati chabe mwatembenuka naku nkala monga kamwana kangóno aka, simuzakangena mu ufumu waku mwamba. ⁴ Chifukwa chake, ali onse wamene azichepesa kunkala monga ka mwana kangóno aka ndiye mukulu mu ufumu waku mwamba. ⁵ Alionse wamene alandila kamwana kangóno monga aka muzina yanga alandila ine. ⁶ Koma ali onse wamene alengesa mwana ali onse wamene akulupilila muli ine kuti achimwe, chawamapo kuti amangiwe kuchi mwala chikulu, naku muponya pansi pa manzi. ⁷ "Soka kuli ziko chifukwa cha vintu vamene vigwesana! Chifukwa nichofunikila kuti vintu vogwesa vibwele, koma soka kuli muntu wamene kugwesana kupitila! ⁸ Ngati kwanja yako kapena kwendo yako ikulengesa kugwa, ijube uyitaye. Chawamapo kuti iwe ungene mu umoyo uli ojubika kapena olemala kuchilapo kuti uponyewe mu mulilo wamene siuzima ukali na manja yabili kapena mendo yabili. ⁹ Ngati linso yako ikulengesa kuti ugwe, ichose uiponye kutali naiwe. Chawamapo kuti iwe ungene mu moyo na linso imozi kuchilapo kuti uponyewe mu mulilo wamene siuzima na menso yako yonse. ¹⁰ Onesesa kuti siusula kamwana kali konse. Chifukwa niku uzani kuti ku mwamba ba ngelo babo bama yangana pa nkope ya ba Tate Banga bamene bali kumwamba. ¹¹ Ma buku yakudala yolemekezeka maningi yalibe aya mau yamene yakamba kuti, "Chifukwa Mwana wa Muntu anabwela kupulumusa chia chamene chinasoba." ¹² Muganizapo bwanji? Ngati muntu ali onse ali na nkosa zokwanila handredi, imozi ikataikapo, samasiya zija zamene zili nainte-naini pa mbali pa chulu naku yenda kukasakila ija yamene yataika? ¹³ Ngati aipeza, zooni nikuuzani kuti, azakondwela maningi pali iyi kuchila pali zija zamene zili nainte-naini zamene sizenze zataika. ¹⁴ Chimozi-mozi, sichifunilo cha ba Tate banu bamene bali kumwamba kuti ali onse pali aba bana bangóno aonongeke. ¹⁵ "Ngati mubale wako akulakwila iwe, enda umuzibise cholakwa chake, pakati kaimwe babili chabe. Ngati amvela, iwe wamu bweza mubale wako. ¹⁶ Koma ngati akana kukumvela iwe, tengako umozi kapena babili boenda nabo kuli eve kuti kupitila mu kamwa ka mboni zibili kapena zitatu liu ili yonse isimikiziwe. ¹⁷ Ngati akana kubamvelela na beve, zibisa baku mupingo. Ngati akana futi kubamvelela baku mupingo, mulekeni uyu muntu ankale monga wa kunja na wamu sonko. ¹⁸ Zooni nikuuzani imwe, vintu vili vonse vamene mumanga pa ziko viza mangiwa kumwamba, na chili chonse chamene muza mangusula pa ziko chizamangusuliwa kumwamba. ¹⁹ Nafuti niku uzani imwe kuti, ngati bantu babili mwagwilizana pa ziko pali chintu chili chonse chamene imwe mupempa, muzapasiwa na ba Tate Banga bamene bali mumwamba. ²⁰ Chifukwa pamene bantu babili kapena batatu bakumana muzina yanga, ine nimapezekapo pakati pabo." ²¹ Pamene apo Petul anabwela naku kamba kuli Yesu kuti, "Ambuye, mubale wanga afunika kunilakwila kangati naine kuti nimukululukile? Mpaka kali seveni?" ²² Yesu anamuyanka kuti, "Ine sinizaku uza kuti kali seveni chabe, koma mpaka ma seveni yali kumi yali nkale seveni. ²³ Mwa ichi ufumu wa kumwamba uli monga mfumu wina wamene anali kufuna kuti aoneselane za malonda naba ntchito bake. ²⁴ Pamene bana yamba kupendelana, wantchito umozi banamuleta wamene anali na nkongole zokwanila ndalama ma teni sauzande. ²⁵ Koma chifukwa chakuti sanali nayo njila yolipililamo nkongole iyi, bwana wake analamula kuti agulisiwe, pamozi na mukazi wake na bana bake na vonse vamene anali navo, kuti nkongole ilipiliwe. ²⁶ Pamene apo wantchito uja anagwa pansi, kugwada pamenso pake, nakukamba kuti, 'Bwana, nipaseniko ntawi, nizalipila zonse nkongole.' ²⁷ Uja bwana wa uja wantchito, chifukwa anamvela chifundo, anamu lekelela naku mukululukila ija nkongole. ²⁸ Koma uja wantchito ana enda nakupeza umozi wantchito munzake, wamene anali na nkongole zake, zokwanila handeledi. Anamugwila, kumukamata pa mukosi, naku muuza kuti, 'Nilipile nkongole yanga.' ²⁹ Koma wantchito muzake uja anagwa pansi naku mupempa, kukamba kuti, 'Nipaseko ntawi, nizakulipila.' ³⁰ Koma uja wantchito oyamba anakana. Koma, anaenda naku mupeleka mu ndende mpaka chabe akalipile nkongole zonse zake. ³¹ Pamene bantchito benangu banzake banaona chamene chinachitika, banakalipa. Banaenda naku uza bwana wabo vonse vamene vinachitika. ³² "Pamene paja bwana wa uja wantchito anamuitana naku muuza kuti, 'iwe wantchito oipa, naku kululukila nkongole zone chifukwa chakuti wenze wanipempa. ³³ Nanga iwe bwanji sunamuchitile chifundo wantchito muzako, monga mwamene ine nenze nakumvelela chifundo?' ³⁴ Bwana wake anakalipa nakumupeleka kuli bomuzunza mpaka pamene azakakwanilisila kulipila nkongole zake zonse. ³⁵ Nichimozi-mozi mwamene ba Tate banga bazachitila kuli imwe ngati imwe pansi pa mutima wanu simu kululukila mubale wanu.

Chapter 19

¹ Pamene Yesu anabwela pambuyo posiliza kukamba aya mau, anachokako ku Galileya nakuyenda kumalo ya Yudeya malo yamene yali kupitilila mumana wa Yodani. ² Magulu yabantu yanamukonka, anabapolesa kwamene kuja. ³ Ba Falisi banabwela kuli eve, kumuyesa, kumuza kuti, "Nanga nichovomelesewa kuti mwamuna asiye mukazi wake palibe chifukwa chili chonse?" ⁴ Yesu anabayanka kuti, "Nanga kansi simunabelenge kuti wamene anabalenga kuchokela kuchiyambi anabalenga mwamuna na mukazi?" ⁵ Eve wamene anabalenga anakamba nafuti kuti, 'chifukwa chake mwamuna azasiya tate wake na mai wake kuyenda kukankala pamozi na mukazi wake, aba babili bazankala tupi imozi.' ⁶ Chifukwa chake sibantu babili manje koma tupi imozi. Chifukwa chake lekani chamene Mulungu aika pamozi, osavomeleza ali onse kuti apatule." ⁷ Banakamba kuli eve kuti, "Nanga nichani kansi chamene Mose anatiuza kuti tikazipasa chi pepala chosiliza chikwati nakumupisha mukazi?" ⁸ Anayanka kuti, "Chifukwa cha kulimba mutima kwanu, ndiye chamene Mose anakuvomelezani kuti musiye bakazi banu, koma kuchokela pachiyambi sichinali njila iyi. ⁹ Nikuuzani imwe, ali onse wamene asiya mukazi wake, kuchoselako chifukwa cha uchiwelewele, ayenda akwatila na mukazi winangu, achita chigololo; nauja mwamuna wamene akwatila uja mukazi osiyiwa achita chigololo." ¹⁰ Bopunzila banamuza Yesu kuti, "Kansi ngati ndiye mwamene chilili pali mwamuna na mukazi wake, sichintu chabwino kukwatila." ¹¹ Koma Yesu anabayanka kuti, "Sibonse bantu bamene bangavomele chipunziso ichi, koma baja bamene bavomelesewa kuti bachivomele. ¹² Chifukwa kuli baja bamene sibafuna chikwatila kuchokela kubadwa kwabo, futi kuli baja bamene sibafuna chikwatila chifukwa cha malamulo yabantu, nafuti kuli baja bamene sibafuna chikwatila chifukwa cha ufumu wa kumwamba. Wamene akwanisa kuchilandila ichi chipunziso, mulekeni achilandile. ¹³ Banaleta bana bang'ono kuti aba ikepo kwanja nakuba pempelela, koma bopunzila bake banabakalipila. ¹⁴ Koma Yesu anabauza kuti, "Bavomeleseni bana bang'ono, osabalesa kuti babwele kuli ine, chifukwa ufumu wakumwamba niwa bantu monga aba." ¹⁵ Anaika manja yake pali bana baja, nakuyenda kuchoka kumalo kuja. ¹⁶ Onani, muntu anabwela kuli Yesu nakukamba kuti, "Apunzisi, nichintu chiti chabwino chamene ine nifunikila kuchita kuti nipasiwe moyo wamene siusila?" ¹⁷ Yesu anamuyanka kuti, "Nanga nichani kansi chamene iwe unifunsila kuti chabwino nichiti? Pali chabe umozi wabwino, koma ngati ufuna kuti ungene mumoyo, sunga malamulo." ¹⁸ Muntu uja anayanka kuti, "Yati malamulo?" Yesu anayanka kuti, "Osapaye, usachita chigololo, usabe, usankale kamboni waboza, ¹⁹ lemekeza batate bako na bamai bako, ukonde muzako monga mwamene uzikondela iwe weka." ²⁰ Uja mwamuna anamuyanka kuti, "Vonse ine nimachita. Nanga kwasala chani chamene nifunika kuchita?" ²¹ Yesu anamuyanka kuti, "Ngati ufuna kuti unkale ofikapo, yenda, kagulise vonse vamene ulinavo, upase bosauka, ndipo uzankala na chuma kumwamba; ubwele, unikonke." ²² Koma pamene munyamata uyu anamvela vamene Yesu anamuza, anaenda omvesana chifundo, chifukwa anali olemela maningi. ²³ Yesu anauza bopnzila bake kuti, "Zoonu nikuuzani imwe, nichintu chovuta kuti muntu olemela angene mu ufumu wakumwamba. ²⁴ Nafuti nikuuzani kuti, nichintu chapafupi kuti Kavalo ingene muka muboó ka nyeleti kuchila kuti muntu olemela angene mu ufumu wa Mulungu." ²⁵ Pamene bopunzila bake banamvela ichi, banali banadabwa kwambili nakukamba kuti, "Kansi nanga nindani wamene angapulumuswe?" ²⁶ Yesu anabalangana nakukamba kuti, "Kuli bantu ichi nichintu chamene sichingakwanilisike, koma kuli Mulungu vintu vonse vikwanilisika." ²⁷ Pamene apo Petulo anayanka kuti, "Onani, tinasiya vintu vonse naku kukonkani. Nanga ise tizapezamo chani?" ²⁸ Yesu anabauza kuti, "Zoonu nikuuzani imwe, mu mubadwe pamene Mwana wa Muntu azakankala pa mupando wake waulemelelo, naimwe bamene munanikonka muzakankala pa mipando zachifumu zili 12, kuweluzi mitundu kumi na zibili zaku Israeli. ²⁹ Ali wonse wamene anasiya manyumba, ba bale, balongo, batate bake, bamai bake, bana, kapena munda chifukwa cha zina yanga azakalandila kupitililapo ntawi zili 100 na kulandila moyo wamene siusila. ³⁰ Koma bambili wamene bali boyambilila bazankala bosilizila, na baja bosilizila bazankala boyambilila.

Chapter 20

¹ Ufumu wakumwamba uli munga mwine wa munda wamene kuseni-seni anaenda kungenesa bantchito kuti basebenzele mumunda wake wa ma gilepsi. ² Pamene ana mvelana nabo bantchito kubalipila ndalama imozi pa siku, anabatuma kuyenda kukasebenza mumunda wake wa mpesa. ³ Ana enda nafuti kuma fili koloko yamu mazulo nakupeza benangu bantchito bali imilile pamalo yamalonda. ⁴ Anabauza kuti, "Naimwe endani mukasebenze mumunda wanga wa mpesa, yamene nizaona kuti ndiye malipilo yanu yabwino ndiye yamene nizakupasani." Pamene apo bana enda kukasebenza. ⁵ Anabwela aendako futi pa ntawi ya twelofu koloko na fili koloko ntawi ya muzuba, nakuchita chimozi-mozi. ⁶ Kamozi futi pantawi ya leveni koloko anaenda nakupeza futi bantu benangu bali imilile banalibe vochita. Anabauza kuti, "Nanga nichani imwe mwaimilila apa kulibe vamenye mungachite?" ⁷ Banamuyanka kuti, "Chifukwa kulibe wamene atingenesa ntchito ise." Anabauza kuti, "Kansi naimwe endani mu munda wanga mukasebenze." ⁸ Pamene inafika ntawi yakumazulo, mwine wa munda uja anauza omulanganila munda kuti, "Baitane bantchito ubapase ndalama zabo." ⁹ "Pamene bantchito baja bamene banangenese nchito pa ntawi ya levini koloko banabwela, ali onse analandila ndalama imozi." ¹⁰ Pamene bantchito baja bamene banayambilila kungena ntchito banabwela, banaganizila kuti beve bazalandila ndalama zambili, koma na beve banalandila ndalama imozi chabe. ¹¹ Pamene banalandila malipilo yabo, banadandaula pali mwine wa munda uja. ¹² Banakamba kuti, "Aba bantchito babwela ntawi yokomboka basebenza chabe ola imozi, koma mwaba folesa chimozi-mozi naise, bamene tasebenza ntchito yolimba yalelo na kupya kwa zuba." ¹³ "Koma mwine wa munda uja anayanka nakukamba kuti, "Muzanga iwe, ine sininakulakwile. Nanga sitenze tamvelana iwe naine kuti muzafola ndalama imozi?" ¹⁴ Ani tenga ndalama yamene iyi ndiye malipilo yako uyende nakuyenda. Ine nasanka kuti na aba bamene bangena ntchito posililiza kuti bafole chimozi-mozi naiwe. ¹⁵ Nanga kansi sinilinzazo mpavu zochita vilivonse na katundu wanga? Kapena uchita nsanje chifukwa cha mutima wanga opasa?" ¹⁶ Chifukwa cha ichi uja muntu osilizila azankala oyamba, uja oyamba ndiye azankala osilizila." Ma buku yochilapo yakudala maningi yalibe aya mau yamene yakamba kuti, "Bambili baitaniwa, koma nibangono bamene basankiwa." ¹⁷ Pamene Yesu anali kuyenda ku Yelusalemu, anatenga bopunzila bake bali kumi na babili pambali, munjila muja nakubauza kuti, ¹⁸ "Onani, apa tiyenda ku Yelusalemu, kwamene Mwana wa Muntu azapelekewa kuli bakulu ba nsembe na bolembe. Bazamuweluzi kuti apaiwe ¹⁹ na kumupeleka kuli bantu Bakunja kuti bamunyoze, bamukwapule, naku mupachika pamutanda. Koma pa siku yachitatu azakaukisiwa." ²⁰ Pamene apo mai wa bana ba Zebediya anabwela na bana bake bamuna. Anagwada pansu pali eve naku pempa chintu. ²¹ Yesu anamuyanka kuti, "Nanga nichani chamene mufuna?" Ana yanka kuti, "Vomelezani kuti bana banga babili aba bakankale, umozi kukwanja yanu yaku manja na wina kukwanja yanu yaku manzele, mu ufumu wanu." ²² Koma Yesu anamuyanka nakukamba uti, "Suziba chamene upempa iwe. Nanga ungakwanise kumwa gome yamene ine nifuna kumwa apa?" Banamuyanka, "Tingakwanise." ²³ Anabayanka kuti, "Gome yanga eeh muzamwa. Koma kunkala ku kwanja yanga ya kwanja na kwanja yanga ya manzele sichintu chakuti ine ningalamule, koma nikwa baja bamene banabakonzela kuli ba Tate banga." ²⁴ Pamene baja bopunzila benangu bali kumi banamvela ichi, banakalipa maningi pali aba babale babili. ²⁵ Koma Yesu anabaitana kuti babwele kuli eve naku bauza kuti, "Imwe muziba kuti basogoleli ba bantu Bakunja bamabafuna kulangiza kuti ndiye basogoleli ku bantu babo, nabaja bantu bozibika bapamwamba bamalangiza mpavu zabo pali beve. ²⁶ Koma kuli imwe visankale njila iyi. Koma, uja muntu wamene afuna kunkala mukulu pali imwe ayenela ankale wantchito kuli imwe, ²⁷ nauja wamene afuna kuti ankale oyamba pakati panu imwe lekani ankale wantchito kuli imwe, ²⁸ munga mwamene Mwana wa Muntu eve sanabwelele kuti bantu bamutumikile, koma kuti atumikile, nakupeleka umoyo wake kunkala cho-ombolelako bantu bambili." ²⁹ Pamene banali kuyena kuchoka ku Yeliko, gulu ikulu inamukonka. ³⁰ Panali ba mpofu babili bamene banali nkale mumbali mwa museu. Pamene banamvela kuti Yesu apita, banapunda kukamba kuti, "Ambuye, Mwana wa Davide, timvelelenikoni chifundo." ³¹ Koma gulu inabakalipila, kubauza kuti bankale chabe ziii, koma beve banapunda mokwezekelatu mau, "Ambuye, Mwana wa Davide, timvelelenikoni chifundo ise." ³² Yesu anaimilila nakubaitana kukamba kuti, "Nanga nichichani chamene imwe mufuna kuti ine nikuchitiline?" ³³ Banamuyanka kuti, "Ambuye, tifuna kuti menso yatu yayambe kuona." ³⁴ Pamene apo Yesu, mogwiliwa nachifundo, anagwila mu menso mwabo. Pamene apo banayamba kuona naku mukonka Yesu.

Chapter 21

¹ Pamene Yesu na bopunzila bake bana fika pafupi na Yelusalemu kumalo ya Betipagi, ku pili ya Oliva, Yesu anatuma bopunzila bake babili, ² kubauza kuti, "Endani mu munzi wamene uli pasogolo, pamene mungena muzapeza ka bulu komangilila, naka mwana kake pamozi. Mutu mangusule mutulete kuli ine." ³ Ngati muntu ali onse akufunsani poni pali twemve, imwe mukambe kuti, 'Ambuye ndiye bamene batufuna,' uja muntu azakulekani kuti mututenge mubwele nato." ⁴ Manje chamene ichi chinachitika kuti vintu vamene anakamba muneneli vikwanilisike. Anakamba kuti, ⁵ "Mu uzeni mwana mukazi waku Ziyoni kuti, 'Ona, Mfumu yako ibwela kuli iwe, Yozichepesa yakwela bulu-pa kamwana ka bulu, ka mwana ka nyama yonyamula katundu'" ⁶ Pamene apo bopunzila banayenda naku chita monga mwamene Yesu anabauzila. ⁷ Banaleta bulu naka mwana ka bulu naku ikapo vovala vabo pali vemve, na Yesu anankala pa vovala. ⁸ Bambili mu gulu banayanzika vovala vabo pa museu, na benangu bana juba tumitengo naku tuika pa museu. ⁹ Pamene apo ma gulu ya bantu yana enda pasogolo pa Yesu na baja bamene banali kumukonka uku ndishi bapunda kukamba kuti, "Hosana kuli mwana wa Davide! Nidalisika wamene abwela muzina ya Ambuye! Hosana kumwamba!" ¹⁰ Pamene Yesu anangena mu Yelusalemu, muzinda one unagwedeseke naku kamba kuti, "Kansi nindani uyu?" ¹¹ Magulu yanayanka naku kamba kuti, "Uyundiye Yesu muneneli wamene achokela ku Galileya." ¹² Yesu anangena mu tempele. Anapisha bonse bamene banali kugulisa naku gula mu tempele, naku pindamula ma tebulo yabaja bochinjisa ndalama na yabaja bamene banali kugulisa nkunda. ¹³ Anabauza kuti, "Chinalembeba kuti, 'Nyumba Yanga izaitaniwa kuti ni nyumba yama pempelo,' koma imwe mwaipanga kunkala nyumba yaba kawalala." ¹⁴ Pamene apo kunabwela ba mpofu na bolemala mu tempele, anabapolesa. ¹⁵ Koma pamene ba bakulu-bakulu nsembe na bolemba bna ona vintu vabwino vamene analikuchita, napamene bana mvela bana bang'ono-bang'ono mu tempele banali kupunda naku kamba kuti, "Hosana kuli Mwana wa Davide," banakalipa maningi. ¹⁶ Banamuza kuti, "Nanga umvela vamene bakamba?" Yesu anabayanka kuti, "Eeeh! Nanga simunabelenge kuti, 'Kuchokela mukamwa mwa bana bang'ono na bana bamene banyonka imwe mwakonzata matamando'?" ¹⁷ Pamene apo Yesu anabasiya nakuyenda kuchoka mumuzinda nakuyenda ku Betani kwamene anagona. ¹⁸ Manje kuseni-seni pamene anabwelela ku muzinda, anamvela njala. ¹⁹ Anaona mutengo wa mukuyu mumbali mwa museu, anaenda kuli mutengo uyu naku peka kuti munali chabe ma tepo. Anau uza mutengo uyu kuti, "Musakankalemo chipaso chilichonse muli iwe futi," na pamene apo uja mutengo unayuma. ²⁰ Pamene bopunzila banaona ichi, bana dabwa nakukamba kuti, "Nanga nichani uyu mutengo wayuma pamene apa?" ²¹ Yesu anabayanka nakukamba kuti, "Zoonu niku uzani imwe kuti, ngati muli na chikulupilo nafuti simukaikila, imwe simuzachita chabe chamene chachitika kuli uyu mutengo wa mukuyu, koma imwe muzakamba na kuli iyi pili kuti, 'Tengewa uyende ukaponyewe mu nyanje,' chamene icho chizachitika." ²² Chili chonse chamene imwe mupempa mu pempelo, mokulupilila, muzalandila." ²³ Pamene Yesu anafika mu tempele, bakulu-bakulu bansembe na bakulu-bakulu ba bantu banabwela kuli eve pamene anali kupunzisa naku kamba kuti, "Nanga nimpavu zabwanji zamene iwe usebenzesa kuchita ivi, nindani wamene anakupasa mpavu zamene izo?" ²⁴ Yesu anabayanka naku kamba kuti, "Naimwe ine nizakufunsani funso imozi. Ngati muzaniyanka, naine nzaku uzani mpavu zamene ine nisebenzesa kuchita ivi vintu." ²⁵ Kubatiza kwa Yohane-kunachokela kuti? Kumwamba kapena ku bantu?" Banakambisana beka-beka, nakukamba kuti, "Apa ngati takamba kuti, 'Kunachokela kumwamba,' eve azati uza kuti, 'Nanga nichani kansi chamene imwe simuna mukulupilile eve?" ²⁶ Koma ngati takamba kuti, 'Ku bantu,' tiyopa gulu, chifukwa bonse bama ona Yohane kunkala muneneli." ²⁷ Banamuyanka Yesu kuti, "Ise sitiziba." Na eve ana bayanka kuti, "Naine sinizaku uzani mpavu zamene ine nisebenzesa kuchita ivi vintu." ²⁸ Nanga imwe muganizapo chani apa? Muntu anali na bana babili. Ana enda kuli uja oyamba naku muuza kuti, 'Mwana wanga, enda ukasebenze mu munda lel.' ²⁹ Uyu mwana anayanka kuti, 'Ine siniza enda,' koma anabwela achinja mutima naku yenda kukasebenza. ³⁰ "Uja muntu anabwela ayenda kuli mwana wake wokonkapo naku muuza chimozi-mozi. Eve anayanka nakukamba kuti, 'Niza enda, atate,' koma sana ende." ³¹ Ni uti pali aba babili wamene anachita chamene ba tate babo banali kufuna?" Bana yanka kuti, "Uja oyamba." Yesu anabauza kuti, "Zoonu niku uzani imwe kuti, baja bamusonko na bachiwelewele bazayambilila kungena mu ufumu wa Mulungu imwe mukalibe kungena." ³² Chifukwa Yohane anabwela kuli mwe minjla yolungama, koma imwe simunamukulupilile. Koma baja bamusonko na bachiwelewele banamu kulupilila. Koma imwe, na pamene imwe muna ona ivi, simuna tembenuke kuti mumukulupilile. ³³ "Mvelani mwambo wina. Kunali muntu, mwine wa munda. Anashanga mpesa, naku ikako chochingilizila, anakumba kotwela mpesa uja, na kumanga nyumba ya olonda, naku ibwelekesa pa ndalama kuli bolima mpesa. Anaenda ku ziko ina." ³⁴ Pamene ntawi yo kolola inafika, anatuma bantchito bake kuli balimi ba mpesa kuti batengeko mbali yake ya mpesa. ³⁵ Koma baja bolima mpesa bana batenga bantchito bake, bana menyapo umozi, bana payapo umozi, naku tema myala wina. ³⁶ Futi, uja

mwine anatuma benangu bantchito bake, bambili bochila baja boyambilila, koma baja balimi ba mpesa bana bachita chimozi-mozi.³⁷ Kuchoka apa, mwine anatuma mwana wake kuli beve, kukamba kuti, 'Mwana wanga bazamuyopa.'³⁸ "Koma pamene baja balimi ba mpesa banaona mwana uja, banakambisana kuti, 'Uyu ndiye azakasala na chuma.' Bwelani, tiyeni timupaye titenge chuma chake.'³⁹ Banamutenga, banamutaya mu munda wa mpesa naku mupaya.⁴⁰ Manje pamene mwine wa munda azakabwela, azakabachita chani baja balimi ba mpesa?"⁴¹ Banamu yanka kuti, "Azaba ononga momvesa chifundo baja bantu boipa munjila yau kali maningi, azabwela abwelekese munda wake kuli benangu balimi ba mpesa, bantu bamene bazamu pasa mbali yake ya vokolola pa ntawi yo enela."⁴² Yesu anabauza kuti, "Nanga imwe simuna belenge mumalemba kuti, 'Mwala wamene baja bomanga bana kana wankala ndiye ogwila nyumba yonse. Ichi chinachokela kuli Ambuye, ndipo nichabwino mumenso yatu'?"⁴³ Chifukwa chake nikamba kuli imwe kuti, ufumu wa Mulungu uzapokewa kuli imwe naku pasiwa kuli ziko yamene izabala vipaso vake.⁴⁴ Ali onse wamene agwelapo pali uyu mwala azapwanyika kunkala tumyala tuong'ono tung'ono. Koma pali ali onse wamene uzagwela aza onongeka."⁴⁵ Pamene bakulu-bakulu ba nsembe na ba Falisi bana mvela izi myambo, banaziba kuti anali kukamba pali beve.⁴⁶ Banali kufuna kuti bamugwile, koma banali kuyopa gulu ya bantu, chifukwa bantu banali kumu kamba kuti ni muneneli.

Chapter 22

¹ Yesu ananena kwaiwo kachibili mumyambi, ndikunena, ² "Ufumu wakumwamba uli munga mfumu inakonzekela pwando yachikwati wa mwana wake mwamuna. ³ Anatuma banchinto bake kuitana bonse bamene banaitaniwa kupwando yachikwati ichi, komanso sibanabwele. ⁴ Nafuti mfumu inaitana banchito bake, nakuti, ' Uzani baja woitaniwa, ' Onani, nakonzeka mugonelo wanga. Ng'ombe yanga natubana twake toina vapaiwa, ndiponso izi zonse nizokonzewa. Bwelani kupwando yaukwati.' ⁵ Koma sianafakileko nzelu ndiponso anayenda, alibonse kuulimi wake, ndiponso wina kumalonda yake. ⁶ Benangu banagwila banchito bamfumu, ndiponso anamvesewa nsoni, nakubapaya. ⁷ Mfumu inakalipa na kutuma basilikali bake, ndiponso banapaya baja bopaya na kushoka muzinda yawo. ⁸ Ndipo anauza banchito bake kuti, 'Chikwati nichokonzekela, koma baja bamene banaitaniwa sibanali oyenela. ⁹ Mwaichi yendani pokumanilana njila ndi kuitana banthu bambili bamene mungakwanise kuitana kupwando yachikwati munga mwamene mungapezele.' ¹⁰ Banchito banayenda munjila, na kusionkana banthu pamozi bonse bamene banapeza, woipa na babwino. Na mumalo yokwatililamo chikwati yanazula na balendo. ¹¹ Koma pamene mfumu inabwela mukati kuona balendo, Inaona mwamuna wamene sanavale zovala vaukwati. ¹² Mfumu inamuuza kuti, ' Munzanga, wabwela bwanji kuno ulibe vovala vaukwati?' Koma uja mwamuna analibe mau. ¹³ Koma mfumu inauza banchito kuti, ' Mumangeni mwamuna uyu kumanja na mendo, ndipo mumutaile panja pofipa, pamene pazankhala kulila nakusheta meno.' ¹⁴ Koma banthu bambili nioitaniwa, koma wosankhidwa nibang'ono." ¹⁵ Ndipo bafalisi banayenda na kukonzekela mwamene bangamugwilile Yesu mumakambidwe yake. ¹⁶ Ndipo banatuma kuli eve bophunzila bake, pamozi nama Herodiya. Banamuuza Yesu kuti, " Muphunzisi, tiziba kuti ndiwe wazooni, na kupunzisa njila za Mulungu . Siumasamalila maganizo ya aliyense, ndipo siulangiza kusanka pa banthu. ¹⁷ Koma tiuze, uganizapo bwanji? kodi nichovomelezewa kupasa musonko kuli kaisala kapena iyai?" ¹⁸ Koma Yesu anaziba kuipa kwawo na kukamba kuti, " Nichifukwa chani chamene muniyesela, imwe bachinyengo?" ¹⁹ Nilangizeni ndalama zamisonko." Ndipo banabwelesa kobili kuli eve. ²⁰ Yesu anakamba kuli beve, " Nanga vili muchifanizilo na zina yabandani ivi?" ²¹ Yesu anabauza kuti, " kaisala." Ndipo Yesu anabauza kuti, " Kansi pasani kuli kaisa zinthu zamene zili za kaisala, ndipo kuli Mulungu zamene zili za Mulungu." ²² Pamene banamvela ivi, banadabwisiwa. koma anamusiya ndikuchokapo ndipo banayenda ²³ Pali ija siku masadusi benangu, bananena kuti kulibe chisinsimuso, anabwela kuli iye. Anamufunsa iye, ²⁴ Nakunena, " Aphunzisi, Mose ananena, ' ngati munthu afa, kopanda mwana, mubale wake afunika kukwatila mukaziwake na kumubalilako mubale wake. ²⁵ Kunali babale bali 7. Oyamba anakwatila na kumwalila. Kosasiyapo mwana aliyense, Anasiya mukazi wake kuli mubale wake. ²⁶ Ndipo mubale wake anachita chimodzimodzi, koma wachitatu, nakufikila kufikila naku mubale wa namba 7. ²⁷ Kuchokela kwa aba onse, mukazi anafa. ²⁸ Manje pakuukisiwa azankhala mukazi wandani pali aba babale bali 7? chifukwa onse anamukwatilapo mukazi uyu." ²⁹ Koma Yesu anayanka ndiponso ananena kwaiwo, "Ndimwe osoba, Chifukwa simuziba malemba olo mphamvu za Mulungu. ³⁰ Koma pachisinsimuso sibamakwatila olo kupasiwa kuchikwati. Koma, ankhala munga angelo kumwamba. ³¹ Koma kulinganiza nazakuukisidwa kwa akufa, simunabelenge zamene zinanenewa kwainu ndi Mulungu, nakunena, ³² ' Kuti ndine Mulungu wa Abulahamu, ndiponso Mulungu wa Isaki, ndiponso Mulungu wa Yakubu?' Mulungu si Mulungu wa akufa, " Koma ni Mulungu wa amoyo." ³³ Pamene magulu inamvela izi, anadabwisiwa ndi kapunzhisidwe kake. ³⁴ Koma pamene afalisi anamvela kuti Yesu abazizilika asadusi, anazikumaniza pamodzi iwo oka. ³⁵ Wina waiwo, okambilako, anamufunsa funso, nakumuyesa_ ³⁶ " Aphunzisi, ni liti lamulo lalikulu pamalamulo?" ³⁷ Yesu ananena kwaiwo, " Konda Mulungu wako namutima wako onse, namoyo wako onse, ndiponso ndi nzelu zako zonse." ³⁸ Iyi ndiye lamulo ikulu yoyamba. ³⁹ Ndiponso lamulo lacibili lili kuti_ ' Konda ozungulila iwe munga mwamene uzikondela.' ⁴⁰ Pali aya malamulo yabili ndiye pamene yonse malamulo ndiponso aneneli ziimilila." ⁴¹ Koma pamene afalisi analipamodzi, Yesu anafunsa funso. ⁴² Ananena kuti, " uganiza chani pali za khristu? Kodi ni mwana wandani?" Ananena kwa iye, " Ni mwana wa Davidi." ⁴³ Yesu ananena kwaiwo, " Chilibwanji, pamene Davidi alimumuzimu pamene amuitana Ambuye, nakunena, ⁴⁴ Ambuye ananena kuli Mulungu wanga, " Nkhala kuzanja lamanja, kufikila napanthawi yamene nizapanga adani ako kunkala pamapazi yako." ⁴⁵ Ngati David amaitana kristhu 'Kuti Ambuye,' Angankhale bwanji mwana wa Davidi? ⁴⁶ Kulibe wamene enze kukwanisa kumuyankha liwu ndiponso kulibe Munthu anayesa kumufunsa mafunso nafuti kuchokela siku ija.

Chapter 23

¹ Pamene apo Yesu anakamba kuuza magulu ya bantu na bopunzila bake. ² Anakamba kuti, "Bolemba na ba Falisi bankala mumupando wa Mose. ³ Chifukwa chake imwe mufunika kumvelela vonse vamene bakuuzani kuti chitani, imwe vichiteni nakuvikonka. Koma musakonke vochita vabo, chifukwa beve bamakamba ivi vintu koma sibamavichita. ⁴ Zo-ona chabe, bamamangilila katundu bolema wamene niwovuta kuunyamula, bamau ika pama pewa ya bantu. Koma beve sibangayese kutandizila nangu naka kumo kamozi chabe kuti banyamuleko. ⁵ Bamachita ntchito yabo kuti bantu babaone. Bamapangisa tuma bokosi toikamo mau ya Mulungu tukulu, nakukulisa vovala vabo kuti baonese monga balemekeza mulungu. ⁶ Bamakonda yaja malo yolemekezeka pa pwando na malo ya ulemu muma Sinagogo, ⁷ na moni bapadela pamalo yamalonda, nakuitaniwa kuti 'Apunzisi' na bantu. ⁸ Koma imwe musaitaniwe kuti 'Apunzisi,' chifukwa imwe muli na mupunzisi umozi chabe, imwe monse ndimwe babale. ⁹ Ndipo musaitane muntu ali onse pa ziko kuti batate, chifukwa imwe muli chabe na ba Tate bamozi, bamene bali kumwamba. ¹⁰ Musaitaniwe kuti 'mupunzisi,' chifukwa muli chabe na opunzisa umozi, Kristu. ¹¹ Koma uja wamene ndiye mukulu pakati panu ankale wantchito. ¹² Ali onse wamene azitukumula aza chepesewa, na uja wamene azichepesa azakwezewa. ¹³ Koma soka kuli imwe, bolemba na imwe ba Falisi, bantu baboza! Mumavala ufumu waku mwamba pa menso pa bantu kuti basangenemo. Imwe bamene futi simungenamo, futi simuvomeleza baja bamene bafuna kuti bangenemo kuti bangene. ¹⁴ Ma lemba yolemekezeka maningi yakudala yalibe aya mau yali mu verse ya nambala 14 (Koma yenangu yamaika iyi vesi pasogolo pa vesi 12). ¹⁵ "Soka kuli imwe, bolemba na ba Falisi, imwe ba mankalidwe yaboza! Chifukwa mumadya muma nyumba ya bazimai bofelewa, mumachita ichi pamene mupempela pempelo itali yakuti imwe muonekele. Chifukwa cha ichi imwe muzalandila kuweluziwa kukulu." Soka kwa imwe, bolemba naimwe ba Falisi, bantu ba mankalidwe yaboza! Muma enda kujumpa nyanja na minda kuti mukatembenule muntu umozi, pamene atembenuka uyo muntu, mumamulenga kunkala kochilapo kabili mwana waku moto monga mwamene mulili imwe. ¹⁶ 'Soka kuli imwe, basogoleli bamene balibe menso, imwe bamene mumakamba kuti, 'Wamene alapa kulapila pa tempele, ichi chilibe ntchito. Koma uja wamene alapila pali golide yamene ili mukati mwa tempele iyi, eve amangiwa na kulapa kwake.' ¹⁷ Imwe basogoleli bopusa bamene balibe menso! Nanga nichiti chikulu, golide kapena tempele yamene ilengesa golide kunkala yoyela? ¹⁸ Na, 'alionse wamene alapila pa guwa, palibe kantu. Koma uja wamene alapila pali chopeleka chamene chilipo, amangiwa na kulapa kwake.' ¹⁹ Imwe ba mpofu! Nanga nichiti chikulu, chopeleka kapena guwa yamene ilengesa chopeleka kunkala choyela? ²⁰ Chifukwa chake, uja wamene alapila pa guwa alapila na vonse vamene vilipo. ²¹ Uja wamene alapila pa tempele alapila pali yeve na uja wamene ankalamo mukati mwake. ²² Na uja wamene alapila kumwamba alapila pamozi na mupando wamfumu wa Mulungu na wamene ankalapo. ²³ Soka kuli imwe, bolemba naba Falisi, bantu ba munkalidwe waboza! Imwe mumapeleka chakumi pali vintu voika kuvakudya, monga sabola, dili na kamini, koma mwasiya vintu vamene vili volema mumalamulo-kuweluziwa na chifuno na chikulupililo. Koma ivi asembe mumachita mosasiya vija vinangu vosachitiwa. ²⁴ Imwe basogoleli ba mpofu, bamene muma kwinyilila pali ka inzi koma muma mela kavalo! ²⁵ "Soka kuli imwe, bolemba na ba Falisi, bamunkalidwe waboza! Chifukwa mumasuka chabe kunja kwa gome nakwa mbale, koma mukati ndimwe bozula na kuzikonda na kuzikondwelesa. ²⁶ Imwe ba mpofu ba Falisi! Sukani poyamba mukati mwa gome na mbale, kuti nakunja kungankale kwabwino nakwemve. ²⁷ "Soka kuli imwe, bolemba naimwe ba Falisi, bamunkalidwe waboza! Chifukwa imwe muli monga choika pa manda, chamene kunja chioneka nichabwino, koma mukati mwake ndimwe bozula na mafupa ya bantu na vonse vintu voipa. ²⁸ Chimozi-mozi, kunja muoneka monga ndimwe bantu bolungama kuli bantu, koma mukati ndimwe bozula na munkalidwe oipa na kusakonka ma lamulo. ²⁹ "Soka kuli imwe, bolemba na ba Falisi, bamunkalidwe waboza! Imwe muma manga manda ya ba neneli naku konza bwino manda ya bantu banali bachilungamo. ³⁰ Mukamba kuti, 'Asembe tinaliko ntawi yama kolo yatu, asembe sitinatengeko mbali muku paya ba neneli.' ³¹ Chifukwa chake imwe mupeleka umboni kuzi weluza pamweka kuti imwe ndimwe bana ba bantu baja bamene banapaya baneneli. ³² Imwe muzulisilatu vamene visasiyako batate banu. ³³ Imwe njoka, imwe bana ba nsato, nanga muzakwanisa bwanji kutaba kuweluziwa kwa ku mulilo? ³⁴ Chifukwa chake, nikutumilani baneneli na bantu banzeli na bolemba. Benangu pali aba muzaba paya naku ba pachika, benangu muzaba menya muma sinagogo yanu nakuba pilikisha kuchoka mumuzinda uyu kuyenda mumzinda winangu. ³⁵ Malipilo yake niyakuti pali imwe pazabwela magazi yonse ya chilungamo yamene yanatikiwa paziko, kuyambila magazi ya Abelo, kufikila magazi ya Zakaliya mwana wa Balakiya, wamene muna paya pakati pa malo oyela na guwa. ³⁶ Zoona nikuuzani kuti, ivi vintu vonse vizabwela pali uyu mubadwe. ³⁷ "Yelusalemu, Yelusalemu, iwe wamene upaya baneneli nakutema myala baja bamene batumiwa kuli iwe! Nikangati kamene ine nafuna kuti ni ike pamozi bana bako, monga mwamene nkuku imaikila pamozi bana bake pansi pama papiko yake, koma iwe siunali kufuna! ³⁸ Ona,

nyumba yako yakusalila yoónongeka.³⁹ Chifukwa nikuuza iwe kuti, iwe siuzakaniona nafuti kufikila pa ntawi yamene iwe uzakakamba kuti niodalisika wamene abwela muzina ya Ambuye."

Chapter 24

¹ Yesu anachoka mu tempele kauyenda njila yake. Bopunzila bake banabwela kuli eve naku mulangiza ma mangidwe ya tempele. ² Koma anabayanka nakubauza kuti, "Nanga simuviona ivi vonse? Zoona niku uzani kuti, kulibe nangu mwala umozi wamene uzasala pamwamba pa wina wamene siuza pwanyika. ³ Pamene anankala pa Pili ya Oliva, bopunzila bake banabwela kuli eve pa beka naku kamba kuti, "Tiuzeni, niliti pamene ivi vintu vizakachitika? Nanga cholangiza kubwela kwanu nichani na cha kusila kwa mubadwe?" ⁴ Yesu anayanka nakukamba kuti, "Nkalani bochenjela kuti muntu ali onse asakutaiseni. ⁵ Chifukwa bantu bambili bazakabwela muzina yanga. Bazakakamba kuti, 'Ine ndine Kristu,' bazakataisa bantu bambili. ⁶ Muzakamvela nkondo na nkani ya nkondo. Onani kuti imwe musavutike, chifukwa ivi vintu viyenela kuchitika; koma kusila kwa ziko sikunafike. ⁷ Chifukwa ziko izakaimila ziko ina, ufumu ufumu wina. Kuzankala njala na kungambika kwa ziko mumalo yosiya-siyana. ⁸ Koma ivi vintu vonse nikuyamba chabe kwa kubaba kwa mumimba yakubeleka. ⁹ Chokonkapo bazakakupelekani ku mavuto naku kupayani. Muzaka zondewa na maiko yonse chifukwa cha zina yanga. ¹⁰ Kukonkapo kwake bambili bazagwa, naku gulisana wina na munzake naku zondana. ¹¹ Baneneli bambili bazakaima naku taisa bantu bambili. ¹² Chifukwa chakuti kupyanya lamulo kuza enda pasogolo, chikondi cha bambili chizaka zizila. ¹³ Koma uja wamene alimbikila mpaka kosilizila azapuluma. ¹⁴ Utenga wabwino wa ufumu uzalalikiwa konse paziko yapansi kunkala mboni kuli maiko yonse. Vokonkapo nikusila kwa ntawi. ¹⁵ "Mwa ichi, imwe mukaona chintu chochitisa nyansa chamene chilengesa kutaya chiyembekezeke, chamene chinakambiwa na muneneli Daniyeli, chili imilile mu malo yoyela" (obelenga amvesese), ¹⁶ "baja bamene bali mu Yudeya lekani batabile kuma pili, ¹⁷ uja wamene ali pa malata ya nyumba asa seluke kuti atengemo kali konse mu nyumba, ¹⁸ nauja wamene ali mumunda asabwelele kuti akatenge chovala chake. ¹⁹ Koma soka kuli baja bamene bali na bana mu masiku yaja! ²⁰ Mupempele kuti kutaba kwanu kusakankale mu ntawi ya mpepo kapena pa Sabata. ²¹ Chifukwa kuzakankala kuvutisiwa kukulu, kuchililatu mwamene kunalili kuchokela pamene ziko inayambila mpaka lelo, kapena kuti vizakachitikako futi iyayi. ²² Asembe aya ma siku siyanachepe sewe, kulibe wamene angapulume. Koma chifukwa cha baja bolungama aya masiku yaza chepesewa. ²³ Ngati muntu ali onse aku uzani kuti, 'Onani, uyu apa Kristu!' kapena, 'Uyo kristu!' musakulupilile. ²⁴ Chifukwa ba Kristu baboza na baneneli baboza bazakabwela naku langiza volangiza vikulu na vodabwisa, kuti bataye, ngati nichokwanilisika, nabaja bolungama. ²⁵ Onani, naku uzani pamene kukali ntawi. ²⁶ Chifukwa cha ichi, ngati baku uzani kuti, 'Onani, ali mu chipululu,' imwe osayendako ku chipululu. Kapena, 'Onani, ali mu chipinda chamukati,' imwe osakulupilila. ²⁷ Mwamene kaleza kaya yakila kuchokela ku mawa kuonekela naku mazulo, ndiye mwamene kuzakankalila kubwela kwa Mwana wa Muntu. ²⁸ Kwamene kuli nyama yakufa, ndiye kwamene kuzankala vikwangala. ²⁹ "Koma pamene kuvutikiswa kuzasila zuba izaka nkala bii, mwezi siuzakapasa ku unika kwake, nyenyezi zizakagwa kuchokela kumwamba, na mpavu zaku mwamba zizaka gwedezeka. ³⁰ Apa manje ndiye pamene kuzakaonekela cho onesela Mwana wa Muntu kumwamba, na mitundu zonse za pa ziko zizaka lila. Bazakamuona Mwana wa Muntu abwela pa makumbi yaku mwamba mwa mpavu na ulemelelo wa ukulu. ³¹ Azaka tuma bangeli bake na kulila maningi kwa lipenga, bazaka ika pamozi balungami bake kuchokela ku mpepo zinai, kuyambila kumbali imozi ya kumwamba mpaka kufikila mbali ina. ³² "Tenganiponi punzilo pali mutengo wa mukuyu. Pamene paja pamene ntambi yake inkala yoteka nakumela matepo, imwe muziba kuti ntawi ya zuba ili pafupi. ³³ Chimozi-mozi, pamene imwe muzakaona ivi vintu vonse, muyenekela kuziba kuti ali pafupi, ali pa chiseko. ³⁴ Zoona niku uzani iwe, uyu mubadwe siuzakapita mpaka ivi vintu vonse vikachitike. ³⁵ Kumwamba na pansu ponse pazakapita, koma mau yanga siyazakapita. ³⁶ Koma kukamba pali siku kapena ntawi kulibe wamene aziba, na bangelo bonse pamozi mali kumwamba, na Mwana, koma ba Tate. ³⁷ Monga mwamene yanalili masiku ya Nowa, chimozi-mozi mwamene kuzankalila kubwela kwa Mwana wa Muntu. ³⁸ Monga mwamene masiku yanalili chikalibe kufika chigumula bantu banali kudya na kumwa, kukwatila na kupelekewa kuchikwati kufikila pamene Nowa anangena mu bwato, ³⁹ sibanazibe kantu kali konse mpaka pamene chigumula chinabwela naku batenga-chimozi-mozi mwamene kuzankalila kubwela kwa Mwana wa Muntu. ⁴⁰ Bamuna babili bazankala mumunda-umozi azatengewa, winangu azasiyiwa. ⁴¹ Bakazi babili bazankala bakutwa na chotwela-umozi azatengewa, winangu azasiyiwa. ⁴² Chifukwa chake, nkalani bochenjela, chifukwa imwe simuziba siku yamene Ambuye banu bazabwela. ⁴³ Koma imwe muzibe ichi, kuti asembe uja mwine wa nyumba anaziba ntawi ya usiku yamene kawalala azabwela, asembe anankala olangana kuonesesa kuti nyumba yake isangenelewe. ⁴⁴ Chifukwa chake imwe mufunikila kunkala bokonzekela, chifukwa Mwana wa Muntu azaka bwela pa ntawi yamene imwe simuyembekezela. ⁴⁵ "Nanga ni uti wamene ndiye okulupililika wamene ba bwana bake baika kulanganila nyumba yabo kuti abapase va kudya pa ntawi yo enela? ⁴⁶ Odalisika ni uja wantchito wamene pamene bwana wake abwela azamupeza akali kuchita ntchito. ⁴⁷ Zoona nikuuzani kuti bwana uja azamu ika

bwana pali chuma chake chamene ali nacho. ⁴⁸ Koma ngati wantchito oipa akamba mumutima wake kuti, 'Bwana wanga achedwa kubwela,'

⁴⁹ ayamba naku menya bantchito banzake, naku mwa nakudya pamozi naba chakolwa, ⁵⁰ uja bwana wake azakabwela pa siku yamene eve saganizila napa ntawi yamene eve saziba. ⁵¹ Bwana wake azakamu juba mu vigaba vigaba naku mupasa malo pamozi nabaja bantu bama nkaliidwe yaboza, kwamene kuzankala kulila naku sheta meno.

Chapter 25

¹ "Ufumu wakumwamba uzakankala monga ba namwali bali kumi bamene banatenga tunyali twabo kuyenda kuti bakakumane naye okwatiliwa. ² Basanu pali aba banali bopusa koma basanu benangu banali bochenjela. ³ Chifukwa pamene banamwali bopusa banatenga tunyali twabo, sibanatenge na mafuta yosebenzesa mu tu nyali twabo. ⁴ Koma banamwali bochenjela bana tenga tu gubu pamozi na tunyali twabo. ⁵ Manje pamene okwatiliwa anachedwa kufika, bamvela tulo naku gona. ⁶ Koma pa kati ka usiku kunali kupunda, 'Onani, okwatiliwa! Endani muka kumane na e. ⁷ Pamene apo bonse baja banamwali banaima naku yasha tu nyali twabo. ⁸ Baja bopusa bana uza bochenjela kuti, 'tipempako mafuta chifukwa tunyali twatu tuzazima.' ⁹ "Koma baja bochenjela banayanka kuti, 'Chifukwa siku zankala yokwanila kuti imwe naise tigabane, imwe endani kuli baja bamene bagulisa mukagule yanu yosebenzesa.' ¹⁰ Pamene bana enda kukagula, okwatiliwa anabwela, na bonse baja bamene banali bokonzekela bana enda na-e kupwando, bana koma nachiseko. ¹¹ "Kuchoka apa manje baja banamwali benangu banabwela nakukamba kuti, 'Bwana, bwana, tisegulileni koni.' ¹² "Koma anabayanka nakukamba kuti, 'Zoonu nikuuzani imwe, ine sinikuzibani imwe.' ¹³ Onesesani, chifukwa imwe simuziba siku kapena ntawi. ¹⁴ "Chifukwa chili monga muntu wamene afuna kuenda kuziko ina. Anabaitana bantchito bake naku bapasa chuma chake. ¹⁵ Kuli umozi anapasa ndalama zisanu, kuli wina zibili, na kuli wina anapasa ndalama imozi. Ali onse analandila zokwanila monga mwamene angakwanilisile, na uja muntu ana enda pa ulendo wake. ¹⁶ Uja wamene analandila ndalama zisanu ana enda pamene apo naku zisebenzesa ndalama zija naku pangilapo ndalama zinangu zokwanila zisanu. ¹⁷ Chimozi-mozi uja wamene analandila ndalama zibili anapangilapo ndalama zinangun zibili. ¹⁸ Koma uja wantchito wamen ealandila ndalama imozi ana enda, naku kumba mugodi, nakubisa ndalama za bwana wake. ¹⁹ Manje pamene panapita ntawi ikulu bwana wa baja bantchito anabwelela naku pendelana ndalama. ²⁰ uja wantchito wamene analandila ndalama zisanu anabwela naku leta ndalama zinangu zisanu. Anakamba kuti, 'Bwana, imwe mwenze munanipasa ndalama zisanu. Onani, ninapangilapo ndalama zinangu zisanu.' ²¹ "Bwana wake anamu uza kuti, 'Wachita bwino, wantchito wabwino okululupilika! Unali okululupilika pa tuntu tung'ono. Apa manje ine nizakupanga o onela vambili. Ngena mu chimwemwe cha bwana wako.' ²² "Wantchito uja wamene analandila ndalama zibili anabwela nakukamba kuti, 'Bwana, imwe munanipasa ndalama zibili. Onani, napangilapo ndalama zibili zinangu.' ²³ Bwana wake anamu uza kuti, 'Wachita bwino, wantchito wabwino okululupilika! Unali okululupilika pali tuntu tung'ono. Niza kuika olanganila vintu vambili. Ngena mu chimwemwe cha bwana wako.' ²⁴ "Pamene apo wanchito uja wamene analandila ndalama imozi anabwela naku kamba kuti, 'Bwana, Niziba kuti imwe ndimwe bolimba mutima. Muma kolola pamene imwe simunashange, ku unjikisa pamene imwe simuna tayepo. ²⁵ Ine ninali na manta, chifukwa chake ine nina enda naku bisa ndalama yanu pansi. Onani, tengani chintu chanu.' ²⁶ "Koma bwana wake anamu yanka naku muuza kuti, 'Iwe wantchito oipa na ulesi, unaziba kuti ine nima kolola pamene sininashange naku unjikisa pamene sinina tayepo. ²⁷ Iwe asembe una bwelekesa ndalama zanga kuli ba malonda ya ndalama, pakubwela kwanga asembe ninapeza ndalama zanga na za pamwamba. ²⁸ Tengani ndalama ili kuli eve mupase uja wamene ali na ndalama kumi. ²⁹ Chifukwa muntu ali onse wamene ali nazo, zambili zinangu zizapasiwa-zopitililapo. Koma uli uja wamene alibe kali konse, navija wamene ali navo azapokewa. ³⁰ Mutayeni panja pamene pali mudima uyo wanchito wamene alibe pindu, pamene kuzankala kulila nakusheta meno.' ³¹ "Pamene Mwana wa Muntu azabwela mu ulemelelo wake na bangelo bonse pamozi na eve, pamene paja azakankala pa mupando wake waulemelelo. ³² Pa menso pake yonse maiko yazaka kumana, ndipo azakapatulula bantu wina kumuchosa kuli wina, monga mwamene mubusa ama patulula nkosa na mbuzi. ³³ Azaika nkosa ku kwanja yake ya kwanja, koma mbuzi zizankala ku kwanja yake ya manzele. ³⁴ Pamene apo Mfumu azakauza baja bamene bali ku kwanj ayake ya manja, 'Bwelani, imwe bamene munadaliska na ba Tate banga, tengani ufumu wamene banaku konzalani kuchokela pamene ziko inalengewa. ³⁵ Chifukwa ine ninali na njala munanipasa bakudya; ninali na njta munanipasa chakumwa; Ninali mulendo munani landila munyumba zanu; ³⁶ Ninali be vovala imwe munani valika; Ninali odwala imwe munanisamalila; Ninali mu ndende imwe munabwela kuniona.' ³⁷ "Pamene apo baja bolungama bazakayanka nakukamba kuti, 'Ambuye, niliti pamene ise tinaku onani njala takusapani vakudya? Kapena na njota takupasani chakumwa? ³⁸ Niliti pamene ise tinakuonani mulendo naku kulandilani? Kapena munalibe vovala nakuku valikani? ³⁹ Niliti pamene tinaku onani kuti mudwala kapena mu ndende naku bwela kukuonani?' ⁴⁰ "Pamene apo Mfumu izakayanka naku kamba kuli beve kuti, 'Zoonu niku uzani imwe, chamene imwe muna chitila mung'ono pali aba babale banga aba, munachitila ine.' ⁴¹ Aza kamba kuli baja bamene bali kukwanja yake ya manzele, 'Chokani apa, imwe botembelelewa, endani mu mulilo wamene unakonzekelwa mudani na bangelo bake, ⁴² chifukwa ine ninali na njala, koma simunani pase vakudya; Ninali na njota, koma imwe simunani pase chakumwa; ⁴³ Nenze mulendo, koma imwe simunani landile mu manyumba yanu; ninalibe

vovala, koma imwe simunani pase vovala; odwala na mu ndende, koma imwe simunani samalile.' ⁴⁴ "Pamene apo baza kayanka nakukamba kuti, 'Ambuye, niliti pamene tenze tinakuonani na njala, kapena na njota, kapena mulendo, kapena osavala, kapena odwala, kapena mundende, ndipo ise siti naku tandizeni?' ⁴⁵ "Azakayanka naku kamba kuti, 'Zoona nikuuzani imwe, vamene imwe simunachitile kuli mungóno pali umozi waba aba, simunachitile ine.' ⁴⁶ Aba bazaka yenda muku kaulisiwa kwamene sikusila, koma balungami bazangena mu moyo wamene siusila."

Chapter 26

¹ Chinabwela chachitika kuti pamene Yesu anasiliza mau yonse, Ananena ku bophunzila bake, ² "Muziba kuti kuchokela masiku awiri Pasaka ilikubwela, ndiponso mwana wa munthu azapelekewa mu kupachikiwa." ³ Ndipo mukulu wabakulu bansembe nabakulu ba banthu banabwela pamodzi mumalo yaopeleka bansembe, wamene analikuitanidwa zina Kayafasi. ⁴ Banapangana kuti bamugwire mobisa ndiponso nakumupaya. ⁵ Chifukwa banalikunena kuti, "Osati nthawi yaphwando chifukwa pangauke chongo pakati pa banthu." ⁶ Manje Yesu anali ku Betaniya munyumba ya Simoni wa khathe, ⁷ pamene anali anasamila pa tebulo, muzimayi wina anabwera kuli eve na botolo ya mafuta yonunkhira ya mtengo wapatali, ndiponso anayitila pamuthu wake. ⁸ Koma pamene bophunzila bake banaona ichi, banabwela bakalipa ndikunena kuti, "Nichifukwa chani ulikuonongela?" ⁹ Sembe mafuta yamene aya yagulisiwa pa mutengo ukulu, ndipo izi ndalama sembe zapasiwa kuosauka." ¹⁰ Koma Yesu, poziba izi, anakamba kuli beve, "Nichifukwa chani muvutisila muzimayi uyu?" ¹¹ Chifukwa achita chinthu chabwino kuli ine. Mumankhala nabosauka nthawi zonse, Koma simuzankhala naine nthawi zonse. ¹² ¹³ Koma pamene anathira mafuta yonunkhira pa thupi langa, achita izi kukonzeka kufwikiliwa kwanga. Nikuuzani zoonza, kulikonse kwamene utenga uzalalikiwa muno muziko, chamene uyu muzimayi achita chizakakambiwapo mukukumbukila uyu muzimayi." ¹⁴ Ndipo umodzi wa kumi na yabiri palibeve oitaniwa Yudas Isikarioti, anapita kuli akulu ansembe nakufunsa kuti, ¹⁵ "Kodi nichani chamene muzanipasa ngati namubwelesa kuli imwe?" Banapima ndalama zokwanila masiliva makumi yatatu. ¹⁶ Kuyambira pamene paja banasakila nthawi yabwino yopeleka Yesu kulibeve. ¹⁷ Pa siku yoyamba yaphwando ya mukate yamene ilibe chotupisa bophunzila banabwela kuli Yesu nakunena ati? "Kodi nikuti kwamene mufuna kuti tikakonzekela malo yodyelamo pasakha?" ¹⁸ Anabauza kuti, "Yendani mumuzinda ku mwamuna wina ndiponso mumuuzi kuti, 'Mupunzisi anena kuti, 'Nthawi yanga yafika. Nizasunga pasakha pa nyumba yako pamozi na bophunzila banga.'" ¹⁹ Bophunzila banachita mwamene Yesu anabauzila, ndiponso banakonzakha chakudya cha Pasakha. ²⁰ Pamene chinafika kumazulo, Yesu anankhala pansi na bophunzila bake khumi na yabiri na kudya. ²¹ Pamene banali kudya, anakamba, "Nikuuzani zoonza imwe kuti umodzi pali imwe azanigulisa." ²² Banamvesewa chisoni, ndiponso wina wache anayamba kumufunsa eve, "Nditu ine sindine, Ambuye?" ²³ Anayankha ati, "Wamene aza ngenesa kwanja kwake pamodzi na ine mubesen ndiye wamene azanigulisa." ²⁴ Mwana wa Munthu azayenda, monga mwamene chinalembedwa pali eve. Koma soka kuli uja munthu wamene azamugulisa! Chinawama ngati uja munthu sanabadwe." ²⁵ Yuda, wamene enzo yenera kumugulisa anati, "Kodi ndine, Mupunzisi?" Anamuza ati, "Wazikambila iwe weka." ²⁶ Pamene benze bakalikudya, Yesu anatenga mukhate, nakuudalisa, ndiponso anaigomola. Anapasako bophunzila bake nakukamba ati, "Tengani, mudyi. Iyi ndiye thupi yanga." ²⁷ Anatenga kapu nakuyamika, ndiponso anabapasa na kukamba ati, "Mwani, imwe bonse." ²⁸ Chifukwa uyu ndiye mwazi wanga wachipangano wamene unatikiwa kukhululuka machimo ya bambiri. ²⁹ Koma nikuuzani, Sinizakamwapa futi ku chipatso cha mutengo wampesa, mpaka siku yamene nizakamwa mwasopano na imwe mu ufumu wa Batate banga." ³⁰ Pamene banaimba nyimbo, banayenda kuphiri ya Olive. ³¹ Koma Yesu anati kuli beve, "Imwe bonse muzagwa usiku uno chifukwa chaine, chifukwa chinalembedwa, 'Nizakwapula mubusa ndiponso nkhoa zizamwazikana.'" ³² Koma pamene nizauka, nizayenda pasogolo painu mu Galileya." ³³ Koma Petulo anakamba kuti, "Chingankhale kuti bonse bagwa chifukwa chaimwe, ine sinizagwapa." ³⁴ Yesu anati kuli eve, "Nikuza zoonza kuti, lelo usiku pamene kombwe akalibe nakulila, uzanikana katatu." ³⁵ Petulo anakamba kuli eve ati, "Chingankhakele kuti ningafele pamozi naimwe, Sinizakukanani." Bonse bophunzila bake banakamba chimodzimodzi. ³⁶ Koma Yesu anayenda na beve kumalo yoitaniwa Getesemani ndiponso anakamba kubophunzila bake, "Nkhalani pamenepano, pamene paja apo, pamene niyenda mukupempela." ³⁷ Anatenga Petulo na bana babili ba Zebedi na eve ndiponso anayamba kunkhala na chisoni na kuvutikiwa mutima. ³⁸ Ndipo anakamba kuli beve ati, "Moyo wanga wazuliwa na chisoni, chakufa nacho. Nkhalani pamenepano ndiponso yanganilani na ine." ³⁹ Anayendanso pang'ono pasogolo, anagwesa nkhoze na kupempela. Anakamba ati, "Tate wanga, ngati nichoteka, lekani iyi kapu inipitilile. Koma, osati kulinganiza nakufuna kwanga, Koma kulinganiza nachifunilo chanu." ⁴⁰ Anabwela kubophunzila bake ndiponso anapeza baligone, ndiponso anauza Petulo, "Nichifukwa chani simunga yanganile na ine ora imodzi?" ⁴¹ Yanganilani na kupempela kuti musagwele mu mayeso. Muzimu ufuna, koma thupi ni yofokela." ⁴² Anayendanso kachibiri mukupempela. Anakamba kuti, "Tate wanga, ngati ichi sichinganipitilile koma chabe nimwe, chifuniro chanu chichitike." ⁴³ Anabwelanso nakupeza bakaligone, chifukwa manso yabo yanali yolema. ⁴⁴ Pamene anabasiyanso, anayenda kupempela ka chitatu, ndikunena mau yamodzimodzi. ⁴⁵ Ndipo Yesu anabwela kubophunzila bake na kubauza ati, "Mukaligone na kupumula? Onani, ora ili pafupi, ndiponso Mwana wa Munthu azagulisiwa mu manja yabochimwa." ⁴⁶ Nyamukani, tiyeni tiyende. Onani, onigulisa alipafupi." ⁴⁷ Pamene enzeli kukamba, Yudas wina wao pali kumi na

abiri, anabwela. Gulu likulu linabwela na eve kuchokela kubakulu bopeleka bansembe ndiponso bakulu ba banthu. banabwela na malupanga na vopumila. ⁴⁸ Manje munthu wamene enzoyenekela kugulisa Yesu anabapasa chizibiso, ndikunena kuti, "Aliyense wamene nizaposhana nakutomola, ndiye wamene muzagwira." ⁴⁹ Pameneapo anabwela kuli Yesu na kukamba ati, "Mulibwanji, Baphunzisi!" ndiponso anamutomola eve. ⁵⁰ Yesu ananena kuli iye, "Muzanga, chita vamene wabwela kuchita." Ndipo bana bwela, kufaka manja pali Yesu, ndiponso banamugwila. ⁵¹ Onani, umodzi pali bamene banali na Yesu anatambusula kwanja kwake, nakudonsa panga yake, ndiponso anakwapula kapolo wa akulu opeleka bansembe, ndiponso anajuba kwatu yake. ⁵² Koma Yesu ananena kuli eve, "Faka panga mumalo yake, chifukwa aliense wamene apaya na lupanga azafa na lupanga. ⁵³ Kodi uganizila kuti asembe sinaitanile Batate banga, asembe sibanitumila ma gulu ya angelo kupambana zikwi khumi na yabiri ?" ⁵⁴ Koma nimunjila yabwanji yamene malemba yazafikilisiwamo, kuti izi zichitike?" ⁵⁵ Pali ija nthawi Yesu anauza gulu ati, "Kodi mwabwela na mapanga na vopumilako nakunitenga monga ndine kawalala? Nenzonkhala lyonse mutempele na kupunzisa, ndiponso simunanimange. ⁵⁶ Koma ivi vonse vachitika kuti malembo ya aneneri yafikilizike." Ndiponso bonse bophunzila banamusiya nakuyenda. ⁵⁷ Baja bamene banamugwira Yesu banamupeleka kuli Kayafasi mukulu wa bansembe, kwamene bolemba na bakulu banakumana pamodzi. ⁵⁸ Koma Petulo anamukonkha mosiyako kamalo kang'ono na nyumba ka mukulu wa bakulu bansembe. Anayenda mukati ndiponso anankhala pansa na bamalonda kuti aone vamene vizachokamo. ⁵⁹ Manje mukulu wa opeleka nsembe ndiponso bonse bamukabungwe banali kuyanganila paukamboni waboza onamizila Yesu, kuti bamupayilepo. ⁶⁰ Sibanapeze aliyense, chingankhale bakhamboni bambiri banabwela pasogolo. Koma pambuyo pake babiri banabwela pasogolo ⁶¹ ndiponso banakamba ati, "Uyu mwamuna anakamba kuti, 'Ningakwanisa kuononga tempele ya Mulungu ndiponso nakuimangana futi muma siku yatatu.'" ⁶² Mukulu wabopeleka nsembe anayimilila no kamba kuli eve ati, "Kodi ulibe yankho? Nanga nichani chamene bapasila umboni pali iwe?" ⁶³ Koma Yesu anankala zii. Mukulu wabopeleka bansembe anakamba ati, "Nakulamilila iwe mwa Mulungu wa moyo, tiuze ngati ndiwe Kristu, Mwana wa Mulungu." ⁶⁴ Yesu anamuyanka ati, "Wakamba ivi wamene iwe. Koma nikuuzani imwe, kuchokela pano muzaona Mwana wa Munthu ankhala kuzanja lamanja la Mphamvu, ndiponso alikubwela pa makumbi ya ku mwamba." ⁶⁵ Ndipo mukulu wa bopeleka bansembe anang'amba zovala zake ndi kunena kuti, "Akamba manyozo! Nichani chamene tikalikusakilila bakamboni? Onani, manje mwamvela manyozo. ⁶⁶ Muganizapo chani?" Banayankha no kamba ati, "Ayenekela kufa." ⁶⁷ Koma banabwela bamutunyila mata kumanso ndiponso kumumenya, ndikumukwapula na kanjeza kumanja yake, ⁶⁸ ndiponso ananena, "Nenelani kuliise, iwe Kristhu. Nanga ni ndani wamene enze kukukwapula?" ⁶⁹ Manje Petulo enze nkhole panja pa malo yanyumba, ndiponso wanchito mukazi anabwela kuli eve nakumuza ati, "Naiwe wenzeli na Yesu waku Galileyo." ⁷⁰ Koma anakana pasogolo pabo bonse, nokamba, "Siniziba vamenekambapo." ⁷¹ Pamene anayenda kunja kwanjila, wanchito wina anamuona ndiponso anauza baja benzepo ati, "Uyu mwamuna naeve enzeli na Yesu waku Nazareti." ⁷² Nafuti anakana ndikulapa, "Sinimuziba!" ⁷³ Pamene kunapita ka nthawi kang'ono baja bamene bana imilila pafupi banabwela nakumuza Petulo ati, "Zooni ndiwe wina wa amodzi aba, chifukwa makambidwe yako yakugulisa." ⁷⁴ Koma anayamba kutembelela na kulapa, "Sinimuziba uyu munthu," ndiponso pameneapo kombwe analila. ⁷⁵ Petulo anakumbuka mau yamene Yesu anakamba, "Pamene kombwe akalibe kulila uzanikana katatu." Ndiponso anayenda panja na kulila kuipa.

Chapter 27

¹ Pamene kunacha, bakulu bakulu bansembe na bakulu bakulu ba bantu bana nkala na maganizo pali Yesu kuti bamu paye. ² Banamumanga, nakumutenga, naku mupeleka kuli Pilato kazembe. ³ Pamene Yudasi, wamene anamupeleka, anaona kuti Yesu bana mu weluza kuti apaiwe, ana tembenuka naku bweza zija ndalama za Siliva zokwanila ma kumi yatatu kuli bakulu bakulu bansembe na bakulu ba bantu, ⁴ naku kamba kuti, "Ine nachimwa chifukwa napeleka magari yamene yalibe mulandu." Koma abanakamba kuti, "Nanga ise tingenamo bwanji? Ziba zako iwe." ⁵ Pamene apo eve anataya pansi zija ndalama mu tempele, naku yenda, naku yenda kukazi mangilila. ⁶ Bakulu bansembe banatenga zija ndalama naku kamba kuti, "Sichovomelesewa kuti ti ike ndalama mu tumba ya tempele chifukwa izi ni mutengo wa magari." ⁷ Banakambisana ichi chintu, nakugula na ndalama izi munda wa opanga mpika kuti yankale manda yoikamo malilo yaba lendo. ⁸ Chifukwa cha ichi uja munda unaitaniwa kuti, "Munda wa Magazi"mpaka na lelo. ⁹ Apa chamene chinakambiwa na Yelemiya muneneli chinafikilisiwa, chokamba kuti, "Banatenga ndalama za Siliva ma kumi yatatu, ndalama za mutengo wamene banamuweluziliwa eve kuli bana ba Izilayeli, ¹⁰ nakugula munda wa opanga mpika, monga mwamene Ambuye banani uzila ine." ¹¹ Manje Yesu anaimilila pamenso pa kazembe, kazembe anamufunsa kuti, "Nanga ndiwe Mfumu ya ba Yuda?" Yesu anamu yanka nakukamba kuti, "Ndiwe wamene ukamba chamene icho." ¹² Koma pamene banamupasa mulandu ba kulu bansembe na bakulu ba bantu, sanaba yanke chili chonse. ¹³ Pilato anamufunsa kuti, "Nanga iwe ndishi siumvela zonse milandu zamene aba bakamba pali iwe?" ¹⁴ Koma sanamuyanike ngakale liu imozi, kulengesa kuti kazembe anankala odabwa maningi. ¹⁵ Manje pa pwando kunali mwambo wakuti kazembe anali ku masula wa mundende umozi wamene anali kusankiwa na gulu ya bantu. ¹⁶ Pa ntawi ija kunali wamu ndende imozi ovuta maningi zina yake Balaba. ¹⁷ Pamene banakumana pamozi, Pilato ana bauza kuti, "Niuti wamene ine nizaku masulilani imwe? Balaba, kapena Yesu wamene aitaniwa Kristu?" ¹⁸ Anaziba kuti banamupeleka Yesu kuli eve chifukwa cha nsanje. ¹⁹ Pamene anali nkezi pa mupando woweluzilapo, mukazi wake anatumiza mau kuli eve kuti, "Imwe musankale na chochita nawo uyo muntu wamene alibe mulandu. Chifukwa ine navutika vintu vambili chifukwa cha chiloto chamene ine ninali nacho pali eve." ²⁰ Manje bakulu bansembe na bakulu ba bantu banalimbikisa gulu kuti ipempelele Balaba, nakuti bamupaye Yesu. ²¹ Kazembe anaba funsa kuti, "Niuti pali aba babili wamene mufuna niku masulileni imwe?" Banayanka kuti, "Balaba." ²² Pilato anabafunsa kuti, nanga uyu muntu Yesu wamene aitanaiwa kuti Kristu nimuchite chani?" Bonse banayanka kuti, "Mupachikeni." ²³ Pamene apo anakamba kuti, "Chifukwa chani, nimulandu wa bwanji wamene apanga?" Koma banapunda mokweza mau kukamba kuti, "Mupachikeni." ²⁴ Pamene Pilato anaona kuti kulibe chamene angachitepo, koma panayamba kunkala pokoso, anatenga manzi, nakusamba kumanja pa menso pa gulu ya bantu, naku kamba kuti, "Ine nilibe mulandu pali magari ya uyu muntu wamene alibe mulandu. Onani wamene muzachuta naye imwe." ²⁵ Bonse bantu banakamba kuti, 'Lekani magari yake yankale pali ise na bana batu." ²⁶ Pamene apo anamu masula Balaba, koma anamukwapula Yesu naku mupeleka kuti apachikiwe. ²⁷ Pamene apo basilikali ba uja Kazembe banamuenga Yesu kuenda naye ku Boma ikulu naku bwelesa pamozi gulu yonse yaba silikali. ²⁸ Banamu chosa vovala nakumu valika mukanjo wofila. ²⁹ Banapanga chisote cha ufumu cha minga naku muika pa mutu, naku mupasa ndondo kumanja yake ya kwanja. Banamu gwadila naku munyoza, kukamba kuti, "Tikuoneni, Mfumu ya ba Yuda!" ³⁰ Banamutunyila mate, naku tenga ndondo naku mumenya pa mutu mobwezelapo. ³¹ Pamene banasiliza kumunyoza, banamuchosa mukanjo naku muvalika vovala vake, nakumupeleka kuti apachikiwe. ³² Pamene bachoka, banapeza mwamuna ochokela ku Saileni zina yake Simoni, wamene banakakamiza kuti aende nabo pamozi kuti amunyamulile mutanda. ³³ Banabwela ku malo yoitaniwakuti Gologota, yamene itantauza kuti "Malo ya Bonzo yaku mutu." ³⁴ Banamupasa vinyo kuti amwe osankaniziwa na ndulu. Koma pamene anayesa kuti amwe, anakangawa. ³⁵ Pamene banamupachika, banagabana vovala vake kupitila muku teya njuga, ³⁶ banankala pansi naku mulonda eve. ³⁷ Pamutu wake bana lembapo mulandu wake, wamene unalembeka kuti, "Uyu ndiye Yesu, mfumu yaba Yuda." ³⁸ Vigabenga vibili vinapachikiwa pamozi na eve, umozi ku kwanja yake ya manja na wina ku kwanja yake ya manzele. ³⁹ Bantu bamene banali kupita banali kumutukwana, uku bapukunya mutu ⁴⁰ nakukamba kuti, "Iwe wamene unali kufuna kuononga tempele naku imanga futi mu masiku yatatu, zipulumuse weka! Ngati ndiwe Mwana wa Mulungu, seluka ubwele pansi kuchoka pa mutanda!" ⁴¹ Chimozi-mozi bakulu bakulu bansembe banali kumunyoza, pamozi na bolemba na bakulu-bakulu, kukamba kuti, ⁴² "Anali kupulumusa benangu, koma eve sakwanisa kuzipulumusa. Eve ndiye Mfumu wa Izilayeli. Mulekeni aseluke abwele pansi pa mutanda, ndiye pamene ise tizamukulupilila. ⁴³ Akulupilila muli Mulungu, mulekeni Mulungu amupulumuse manje apa, ngati Mulungu avomela kumu masula. Chifukwa ana kamba kuti, 'Ine ndine Mwana wa Mulungu.'" ⁴⁴ Chimozi-mozi vigabenga vija wamene vinapachikiwa pamozi na eve vina munyoza. ⁴⁵ Manje kuchokela ntawi ya twelve koloko

yamu zuba kufikila ntawi ya fili koloko yamu zuba kunankala chimudima pa ziko yonse.⁴⁶ Pa ntawi ya 3 koloko yamu zuba, Yesu anapunda na liu yokweza naku kamba kuti, "Eli, ELi, lama sabakatani?" kutantauza kuti, "Mulungu wanga, Mulungu wanga, nichani chamene mwanilekelela ine?"⁴⁷ Pamene baja bamene banali imilile banamvela ichi, banakamba kuti, "Aitana Eliya."⁴⁸ Pamene apo umozi pali baja ana enda naku tenga tonje, aizulisa na vinyo vosasa, ai ika pa ndondo ya nente, nakumupasa kuti amwe.⁴⁹ Bonse bamene banasala banakamba kuti, "Musiyeni eka. Lekani tione ngati Eliya azabwela kuti amupulumuse."⁵⁰ Pamene apo Yesu analila na liu yokweza naku peleka muzimu wake.⁵¹ Onani, chinyula chogabisa tempele china ngám-bika pakati kuyambila kumwamba kufikila pansi, na ziko inagwedezeka, na myala zina ngám-bika.⁵² Manda yana seguka, ma tupi ya bantu boyela bamene bana gona yanaukisiwa.⁵³ Bana choka mu manda pamene eve anaukisiwa, naku ngena mu muzinda oyela, naku onekela kuli bambili.⁵⁴ Manje pamene Kentuliyo pamozi nabaja bamene banali kuona Yesu banaona kungambika kwa ziko na vintu vamene vinachitika, banayopa nakukamba kuti, "Zoonu uyu anali Mwana wa Mulungu."⁵⁵ Bazimai bambili bamene banakonka Yesu kuchokela ku Galileya kumusamalila banaliko kulanganila patali.⁵⁶ Pali aba panali Maria Madalena, Maria mai wake wa Yakobo na Yosefe, na mai wa bana ba Zebediya.⁵⁷ Pamene kunakala mazulo, kunabwela mwamuna olemela ochokela ku Alimatiya, zina yake Yosefe, wamene anali opunzila wa Yesu.⁵⁸ Anafika kuli Pilato naku pempa tupi ya Yesu. Pamene apo Pilato anabauza kuti bamupase.⁵⁹ Yosefe anatenga tupi, kui vumbatila mu nyula yo tuba,⁶⁰ naku iika mumanda yake yamanje yamene ana kumba mu mwala. Pamene apo anaika chimwala chikulu pa komo ya manda naku enda.⁶¹ Maria Madalena na uja Maria winangu banaliko kuja, banali nkale kulangana manda.⁶² Siku yokonkapo, yamene inali siku yokonka siku Yokonzekela, bakulu-bakulu ba nsembe na ba Falisi banali banakumana pamozi na Pilato.⁶³ Banakamba kuti, "Bwana, ise tikumbukila kuti uyu muntu waboza pamene anali na moyo, anali anakamba kuti, 'Pakapita masiku yatatu nizauka futi.'"⁶⁴ Chifukwa cha ichi imwe lamulani kuti manda baya londe kufikila siku ya chitatu, ndaba bopunzila bake bangabwele nakuba tupi yake naku yamba ku uza bantu kuti, 'Auka kubakufa,' na kunamiwa kosilizila kuzankala kukulu kuchilapo paja poyamba."⁶⁵ Pilato anabauza kuti, "Tengani malonda. Endani mukaonesese kuti manda yalondewa munjla mwamene imwe mungakwanilisile."⁶⁶ Pamene apo banayenda naku londesa manda, kuvala chimwala naku ikapo bolonda.

Chapter 28

¹ Manje paku yenda kusila kwa Sabata, pamene kunayamba kucha siku yo yamba ya Sabata, Maria Madalena na uja Maria wina bana bwela kumanda. ² Onani, kunali kungambika kwa ziko, chifukwa mungeli wa Mulungu anaseluka kuchokela kumwamba, nakubwela kuchosapo chimwala, naku nkalapo pachimwala. ³ Anali kuoneka monga kaleza, na vovala vake vinali votuba monga matalala. ⁴ Bolonda bana njenjema na manta naku nkala monga bantu bakufa. ⁵ Mungeli ana kamba nabo bazikazi naku bauza kuti, "Musayope, chifukwa ine niziba kuti musakila Yesu, wamene anapachikiwa. ⁶ Salipo pano, koma aukisiwa, monga mwamene anakambila. Bwelani muone pa malo pamene Ambuye banagona. ⁷ Endani mwa musanga muka bauze bopunzila bake kuti, 'Aukisiwa kubakufa. Onani, aenda akusogolelani kuyenda ku Galiyeya. Kwamene kuja muzamuona.' Onani, naku uzani." ⁸ Bakazi baja banachokako kumanda mwamusanga na manta mo kondwela kukulu, naku tamanga kuti bakauze bopunzila bake. ⁹ Onani, Yesu anaba kumana naku bauza kuti, "Moni!" Bazikazi banabwela, nakugwila mendo yake naku mupembeza. ¹⁰ Yesu anabauza kuti, "Musankale na manta. Endani mukabauze babale banga kuti bachokeko ku Galileya. Kwamene uja bazaniona." ¹¹ Manje pamene bakazi banali kuyenda, onani, benangu pali bamalonda bana enda mumuzinda naku uza bakulu-bakulu bansembe vintu vonse vamene vinachitika. ¹² Pamene ba nsembe banakumana na bakulu bakulu naku kambisana pali ichi chintu na beve, bana pasa ndalama zambili maning kuli ba silikali ¹³ naku bauza kuti, "Benangu mubauze kuti, 'Bopunzila ba Yesu benze bana bwela usiku ndishi ise tili gone nakuba tupi yake.' ¹⁴ Ngati iyi nkani yafika kuli ba kazembe, ise tizakamba nabo kuti imwe musa vutike mutima." ¹⁵ Mwa ichi baja basilikali bana tenga ndalama naku chita monga mwamene bana bauzila. Iyi nkani ina pelekewa maningi kuli ba Yuda bambili ndipo yapitiliza kufikila mpaka lelo. ¹⁶ Koma baja bopunzila banali kumi na umozi bana enda ku Galileya, ku pili yamene Yesu anabauza. ¹⁷ Pamene banamuona, banamupembeza, koma benangu banakaikila. ¹⁸ Yesu anabwela kuli beve naku bauza kuti, "Zonse mpavu zapasiwa kuli ine kumwamba na pansu. ¹⁹ Endani imwe muka pange bopunzila mu maiko yonse. Muba batize mu zina ya ba Tate, ya Mwana, na ya Muzimu Oyela. ²⁰ Mubapunzise kuti bamvele vintu vonse vamene ine nina kuuzani. Onani, Ine nili naimwe ntawi yonse, mpaka kufikila kosilila ntawi."

Mark

Chapter 1

¹ Ici ndiye ciyambi ca nkani yabwino ya Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu. ² Monga vinalembewa na Mneneri Yesaya, "Onani nituma Kapaso wanga pamenso panu, wamene azakonzana njila yano. ³ Mau ya uyo opunda msanga, 'Konzani njira ya Ambuye; mupangileni njila ilibe makona.' ⁴ Yohane anabwera, nakubatiza msanga nolalikila za ubatizo olapa paku khululukidwa kwa macimo. ⁵ Ziko yonse ya Yudeya na anthu onse aku Yerusalemu anayenda kuli yeve. Anabatiziwa na eve mumana wa Yolodani, nakuvomela macimo yawo. ⁶ Yohane anzovala zovala zausako wa ngamila na beluti ya cikumba mumsana mwake, ndipo anali kudya nthete na uchi wamusanga. ⁷ Analalikila, "Winangu alikubwela pambuyo panga wamene ali wamphavu kupambana ine, ndipo sindiyenela kubelama kumangusula ntambo yansapato zake. ⁸ Ine nikubatizani na manzi, koma iye azakubatizani imwe na Mzimu Woyela." ⁹ Vinacitika ivi mumasiku aja pamene Yesu acacokera ku Nazaleta mu Galileya, ndipo anabatiziwa na Yohane m'mumana wa Yolodani. ¹⁰ Pamene Yesu anacoka mumanzi, anaona kumwamba kwa seguka na Mzimu ulikuseluka mowoneka ngati kunda. ¹¹ Na mau anacokela kumwamba nati, "Ndiwe mwana wanga wenikonda. Ndi kondwela nawe." ¹² Ndipo Mzimu unampeleka yeve kuyenda kusanga. ¹³ Enze msanga kwa masiku 40, kuyesewa na satana. Anali na nyama za msanga, na Angelo kumtumikila eve. ¹⁴ Manje pamene Yohane anamangiwa, Yesu anabwele ku Galileya alikulalikila uthenga wa Mulungu, ¹⁵ elo enzokamba ati, "Nthawi yakwana, ndipo ufumu wa Mulungu uli pafupi. Lapani ndipo mkhulupilile mu uthenga." ¹⁶ Pamene enzokuyenda mumbali mwa kamana ka Galileya, anaona Simoni na Anduleya mbale wa Simoni alikukuponya kombe muchimana, cifukwa anali ogwira nsomba. ¹⁷ Yesu anabauza ati, "Bwelani, nikonkheni, ndipo ndizakupangani ogwira anthu." ¹⁸ Ndipo pamene apo anasiya makombe nomukonkha. ¹⁹ Pamene Yesu anayendako cabe pang'ono, anaona Yakobo mwana wa Zebediya na Yohane mbale wake; anali muboti alikutunga makombe. ²⁰ Anabaitana ndipo anasiya Atate awo Azebediya na a nchito muboti, nakumukonka. ²¹ Ndipo anafika ku kapenamu, ndipo pa sabata, Yesu anangena musunagoge nophunzisa. ²² Anadabwa navenzeli kuphunzisa, analikuphunzisa ngati munthu anali na ulamuliro osati nga na alembi. ²³ Pamene apo munali munthu

musunagoge enze na mizimu yoipa yamene inalila ²⁴ nati, "Nanga tinambali bwanji naiwe, Yesu waku Nazareti? Wabwela kutiononga? Nikuziba iwe. Niwe woyela wa Mulungu!" ²⁵ Yesu anakalipila dimoni nati, " Siya kukamba ndipo coka mwaiye!" ²⁶ mzimu woipa unamgwesa pansi nakucoka mwa iye ulikulila mokuwa. ²⁷ Ndipo anthu wonse anadabwa, ndipo anafunsana wina ndi muzake, " Nanga ici nicani? Ciphunziso casopano cina ulamulilo? Alamulila na mizimu yoipa ndipo imumvelela!" ²⁸ Mbili yake inamveka pali ponse mumzinda wonse wa ku Galileya. ²⁹ Pamene anacoka musunagoge, anangena munyumba ya Simoni na Andeleya pamodzi na Yakobo na Yohane. ³⁰ Manje apongozi a Simoni enze gone odwala mphepo, anamuuza Yesu za iye. ³¹ Ndipo Yesu anabwela, anamugwila pa kwanja , nakumunyamula; mphepo inacoka, ndipo anayamba kubapasa vakudya. ³² Mazulo mwake, pamene zuba inangene , anabwelesa kwake wonse odwala nabamene enze naviwanda. ³³ Muzinda wonse unasonkhana panja pa ciseko. ³⁴ Anacilisa ambiri enze odwala matenda wosiyana-siyana nocosa madimoni ambiri, koma sanavomeleze madimoni kuti yakambe cifukwa yanamuziwa iye. ³⁵ Anauka kuseni-seni, kukali kofipa; anacoka nakuyenda kumalo kwayeka ndipo anapemphela kwamene kuja. ³⁶ Simoni na aja enze naye anamusakira. ³⁷ Anamupeza nakumuuza kuti, "Anthu wonse asakila iwe." ³⁸ Iye anati, "Tiyeni tiyende kwina, kumizinda inangu, kuti nikalalikileko nakweve. Nicifukwa cake nina bwela kuno." ³⁹ Anayenda malo yonse ya Galileya, kulalikila mumasunagoge yawo nakucosa madimoni. ⁴⁰ Munthu wolwala makate anabwela kwa yeve. Anali kupempha iye; anagwada pansi nakuti, "Ngati mufuna, munganitubise" ⁴¹ Yesu anamvela cifundo, nakumugwila nakwanja kwake nati, "Ndifuna, kuyelesewe." ⁴² Pamene apo makate anacoka iye, ndipo anapola. ⁴³ Yesu anamucenjeza maningi nakumuuza ati ayende ⁴⁴ Anati kwa yeve, "usayese kuuza munthu aliyense, koma yenda ukazilangize kwa wansembe, ndipo ukapeleke nsembe yakukuyelesela ija yamene analamulila Mose, ngati umboni kwa beve." ⁴⁵ Koma anayenda nayamba kuuza aliyense nopeleka nkhani nopangisa kuti Yesu asakwanise kungena momasuka m'muzinda uliwonse. Ndipo anankhala ku malo kunalibe anthu enzonzhalako ndipo anthu anabwela kuli eve kucokela kosiyanasiyana.

Chapter 2

¹ Manje pamene anabwelako ku kapenamu, patapita pa masiku yang'ono, inamveka mbili kuti ali panyumba. ² Ndipo ambili anabwela kwamene anali kuti malo yonse yanazula, na pa komo ponse, ndipo Yesu analankhula nawo mau. ³ Ndipo amuna ena anabwela kwa iye ananyamula mwamuna wozizila mubili, Amuna anai anamunyamula iye. ⁴ Pamene analepela kufika pafupi ndi iye cifukwa ca nyamutindi wa anthu, anapasula mutenje wanyumba pamene analili. Ndipo anakumba zenje, anaingenesa mpasa pamene panali munthu wozizila mubili. ⁵ Pakuona chikhulupirilo cawo, Yesu anati kwa uja wozizila mubili, " Mwana wanga, macimo yako yakhululukiwa. ⁶ "Manje alembi ena enze anali nkale pamene paja, banaganiza mkati mwamitima yawo, ⁷ "Uyu anagakambe bwanji telo? Alikonyozela! Ndani angakululukile macimo koma Mulungu cabe? ⁸ Yesu ananziba mwamusanga m'mzimu wake vamene benzoganiza, Anati kwa iyo, "Cifukwa nicani mulikuganiza motelo mmitima yanu? ⁹ Capafupi nicabwanji kunena kuli wozizila mubili kuti, 'Macimo yako yakhululukiwa' kapena kulankhula kuti 'Ima, Tenga mpasa yako, yenda?' ¹⁰ Koma kuti muzibe kuti mwana wa Munthu ali ulamulilo pa dziko yapansi yokhululukila macimo, "anati kuli uja wozizila mubili, " ¹¹ Nikuti kuli iwe, ima, tenga mpasa yako, pita kunyumba kwako." ¹² Anayima pamene apo, nakuthenga mpasa nakuyenda ku nyumba kwake pakazanga ka anthu, ndipo wonse anadabwa ndi kupeleka ulemelero kwa Mulungu, nati, "Tenze tikalibe kuonapo vya so." ¹³ Anayendanso pa chimana, ndipo anthu wonse anaza kwa iye, ndipo anabaphunzitsa. ¹⁴ Pamene ali kupita anaona Levi mwana wa Alefa alinkhale posonkhela msonkho ndipo iye anati, "Unikonkhe ine" anaima nakumukonkha iye. ¹⁵ Ndipo pamene Yesu anali kudya munyumba ya Levi, ambiri wosonkhesa msonkho ndi wocimwa banali kudya naye Yesu ndi wophunzila ake, chifukwa anali ambiri amene anali kumukonkha. ¹⁶ Pamene alembi, amene anali Afalisi, anaona kuti Yesu anali kudya pamodzi ndi wocimwa ndi wosonkhesa msonkho, anati kwa wophunzila ake, "Chifukwa nicani ali kudya pamodzi ndi wosonkhesa msonkho ndi anthu wocimwa?" ¹⁷ Pamene Yesu anamvwa izi anati kwa iwo, " Anthu wolimba mthupi samafuna dokotala; koma iwo amene ali wodwala amafuna dokotala. Sindinabwele kuzoitana anthu wolungama, koma anthu wocimwa." ¹⁸ Wophunzila a Yohane ndi Afalisi anali kusala kudya. Ndipo anthu ena anaza ndikunena kwa iye, " Chifukwa nicani wophunzila a Yohane alikusala kudya, koma wophunzila anu salikusala kudya?" ¹⁹ Yesu anati kwa iwo, "Kodi wobwela ku cikwati angasale kudya pamene mwine ukwati ali nawo pamodzi? maka-maka ngati mwine wa ukwati alipo sangasale kudya. ²⁰ Koma masiku yazabwela pamene mwine ukwati azatengedwa pakati pawo, pamasiku ayo, azakasala kudya. ²¹ Palibe amene amasokha nyula yanyowani pa cigamba ca kale, ngati acita telo cigamba cizang'ambika, canyowani cizang'amba ca kale, ndipo cizang'amba kwambiri. ²² Kulibe amene amaikha vinyo wa lombamba muthumba ya vinyu yakale, ngati acita telo thumba ya vinyu ipulike ndipo zonse vinyu ndi thumba ya vinyu izaonongeka. Cofunika ni kuika vinyu wa nyowani mu thumba ya vinyu ya nywani." ²³ Pa siku ya Sabata Yesu analikupita pakati ka munda wa tiligu, ndipo wophunzila ake anayamba kutyola mitu ya tiligu. ²⁴ Ndipo Afalisi anati kwa iye, " Onani, Chifukwa nicani alikucita zamene lamulo la sabata silivomeleza?" ²⁵ Iye anati kwa iwo, "Kodi simunabelengepo zamene Davide anacita pamene anali ndi njala ndi kufunisisa kudya - ndi anthu amene anali naye- ²⁶ mwamene anayendela mu nyumba ya Mulungu pamene Abithala anali Mkulu wansembe, ndipo anadya buledi ya mkati, camene sicinali covomelekedwa ku munthu aliyense kocoselako cabe wansembe, ndipo iye anapasako ndi iwo amene anali nawo?" ²⁷ Yesu nati, " Sabata niya munthu osati munthu ankhale kapolo wa sabata. ²⁸ Chifukwa cake, mwana wa Munthu ni mbuye wa Sabata."

Chapter 3

¹ Mobwezela anangenanso musinagoge munali mwamuna anali ndi kwanja yofota. ² Benangu banthu banali kumuyang'ana kuti baone ngati azamupolesa pa sabata kuti bamupase mulandu. ³ Yesu anati kuli uja munthu wofota kwanja, "Ima, Imilila pakati pa wonse." ⁴ Ndipo anati ku banthu, "Kodi nichovomelekezeka kucita chabwino pa siku ya Sabata kapena kuchita chinthu choyipa; kupulumusa moyo, kapena kupaya?" Ndipo wonse banali chete. ⁵ Anabayangana naukali, na kumudwisiwa na kuuma mutima kwawo, ndipo anati kumwamuna, "Tambulula kwanja kwako." Ndipo iye anatambulula, na kwanja kwake kunankhala bwino. ⁶ Bafalisi panthawi yamene iyo banapita kukafuna-funa njila yomupailamo pamodzi nama Helodiya. ⁷ Ndipo Yesu, pamozi na wophunzila, banayenda kunyanja, ndipo banthu bambili banamukonkha kucokela ku Galileya ndi ku Yudeya ⁸ na kucokela ku Yelusalemu naku Idumeya nakupitilila Yorodani na kuzungulila Tireya na Sidoni. Pamene ananva pa zamene analikucita, banthu bambili banabwela kuli eve. ⁹ Ndipo anafunsa wophunzila bake kuti bakonzeke kaboti kang'ono chifukwa banthu banali bambili, kuti osati bazimuguma-guma. ¹⁰ Chifukwa anachilisa bambili, kuti aliyense wamene anali wovutika anafuna-funa kuti afike kuli eve kuti amugwileko. ¹¹ Nthawi zonse pamene mizimu yoipa unamuona eve, unalikugwa pansi na kulila kokuwa, nakukamba kuti, "Iwe ndiwe Mwana wa Mulungu." ¹² Ndipo iye anali kukulesa kuti asamuzibe. ¹³ Anayenda palupili, na kuyitana baja bamene anali kufuna, ndipo banabwela kuli eve. ¹⁴ Anasankhapo bali 12, (bamene anaitana kuti apositolo), kuti bazinkhala naye ndipo akabatume kukalalikila uthenga. ¹⁵ na kunkala na mpamvu zochosela vibanda. ¹⁶ Ndipo anasankhapo 12: Simoni, wamene anapasa zina yakuti Petulo; ¹⁷ Yakobo mwana wa Zebedayo, and Yohana mu mbale wa Yakobo, kuli awo anapasa zina Bonenge, kuthanthauza Bana baka kaleza; ¹⁸ na Andileya, Filipino, Batolomeyo, Mateyo, Tomasi, Yakobo mwana wa Afalesi, Thadeyo, Simoni wa Zilote, ¹⁹ na Yudasu Iscariyoti, uja wamene anamugulisa. ²⁰ Ndipo anayenda kunyumba, na banthu bambili banabwela pamozi futi, kuti bakane kudya buledi. ²¹ Pamene babanja bake bananvaa ivi, banayenda kuti bakamugwile, cifukwa anati, "aleka kuganiza bwino." ²² Balembi bamane banabwela kucokela ku Yelusalemu anati, "ali na vibanda vya Beluzabebu," ndipo, "mwa ulamulilo wa vibanda ochosa vibanda," ²³ Yesu anabaitana na kubauza mu myambi, "Zingachitike bwanji kuti Satana achose Satana? ²⁴ Ngati ufumu niwogabanikana suungaimilile. ²⁵ Ngati nyumba niyogabanikana, ija nyumba siingaimilile. ²⁶ Ngati Satana aziukila eka na kugabanikana, sangaimilile, koma kwabwela kusila. ²⁷ Koma palibe amene angangene munyumba ya wampamvu nakuba vonse vauja munthu bakalibe kumumangilila, ndiye pamene bangaononge nyumba yake. ²⁸ Zoona nikuuzani, uchimo uliwonse wa mwana wa munthu uzakakhululukidwa, na minyozo yonse yokambiwa, ²⁹ koma aliwonse wonyoza Muzimu Woyela sazakhululukiwa, koma azankhala wochimwa ndi uchimo wa nthawi zonse." ³⁰ Yesu anakamba izi chifukwa banali kukamba kuti, "Ali na mizimu yonyansa." ³¹ Ndipo bamai bake na babale bake banabwela nakuimilila panja. Banatuma banthu, nakumuitana. ³² Ndipo banthu bambili banalipo nankhala momuzungulila iye na kuti, "Bamai bako na babale bako bali panja, dnipo bakufuna," ³³ Anabayankha nakuti, "Nibandani bamai banga na babale banga?" ³⁴ Anabalangana baja bamene banali nkhole banamuzunguluka nakuti, "Onani, aba ndiye bamai banga na babale banga! ³⁵ Chifukwa aliwonse wamene achita chifunilo cha Mulungu, uja munthu ndiye mubale wanga, na mulongo ndi mai wanga."

Chapter 4

¹ Nafuti anayamba kuphunzitsa mumbali ya chimana. Ndipo anthu ambiri anaza kwa iye, ndipo anasika mu boti inali pachimana, nakhala pansi. Anthu wonse anali kumbali kwa chimana. ² Anabaphunzisa zinthu zambiri mumafanizo, ndipo anati kwawo muciphunzinso, ³ Mvelani, mlimi anayenda kukafesa mbeu zake. ⁴ Pamene analikubyalala, mbeu zina zinagwela munjila, mbalame zinabwela nakudya mbeu. ⁵ Mbeu zina zinagwela pamwala, panalibe doti yambili. Nthawi yamene zinangomela, cifukwa mizyu siinayende kwambili pansi pa doti. ⁶ Koma pamene zuwa inacoka, zinapya, cifukwa zinalibe mizyu zinayuma. ⁷ Mbeu zina zinagwela mitengo ya minga. Mitengo ya minga inakula ndipo mbeu inalasidwa, ndipo siinabale mbeu iliyonse. ⁸ Mbeu zina zinagwela panthaka yabwino ndipo zinabala zipaso pamene zinali kukula ndikukuluka, zina zinabala makumi yatatu (30), zina makumi asanu ndi imodzi (60), ndi zina makumi kumi (100)." ⁹ Ndipo anati, "uyo ali ndimakutu omvela, amve!" ^{10 11 12} Pamene Yesu anali yeka, iwo amene anali naye pafupi ndi iye ndi aja twelufu anamufunsa iye za fanizo. Ndipo anati kwawo, "kuli imwezapasidwa zisinsi za ufumu wa Mlungu. Koma kwa iwo ali kunja zonse zili mumafanizilo, kuti pamene apenya, inde azapenya, koma sazaona, ndipo pamene azamva, inde zamva, koma sazamvesa, kuti angabwelele kuli Mlungu ndikubakhululukila macimo yawo." ¹³ Ndipo anati kwa iwo, "Simvesesa fanizo iyi? Muzamvesesa bwanji mafanizo yena?" ¹⁴ Mlimi amaene anafesa mbeu yake ndiye amane afesa mau. ¹⁵ Zina zimene zinagwela mbali mwa njila, mwamene mau anagwela. Ndi pamene amvela mau, Satana panthawi yamene iyo amabwela ndikutenga mau amene anafesedwa mwa iwo. ¹⁶ Ndi zina zimene zinafesedwa pa mwala, ndi iwo amene amamva mau, nthawi yamene amalalikidwa mau amalandila ndi chimwemwe. ¹⁷ Ndipo alibe mizu mwa iwo, koma amalimbikila kwa kathawi kocepa. Pamene akumana ndi mabvuto kapena abanzunza cifukwa ca mau nthawi yamene ija amagwa. ^{18 19} Ndipo zina zamene zinagwela pa minga. Amamva mau, ¹⁹ koma nkhwawa ya zamudziko, chinyengo ca vya cuma, cilakolako ca vinthu vina cimabangena, cimaononga mau, ndipo amankhala opanda cipatso. ²⁰ Ndipo zina zinja zamene zinafesedwa pa nthaka yabwino. Iwo amamva mau ndikulandila ndikubala zipatso; zina makumi yatatu(30) ndi zina makumi asanu ndi imodzi(60) ndi zina makumi kumi (100) ²¹ Yesu anati kwa iwo, "Kodi mungabwelese nyali mukati mu nyumba naku iika pansi pa basiketi kapena pansi pa bedi? Muzailleta mukati naku iika poika nyali. ²² Chifukwa kulibe chamene nichobisika chamene sichizazibika, ndiponso kulibe chamene chili chosazibika chamene sichizabwela po-onekela. ²³ Ngati wina ali onse ali na matu yomvelela, lekani amvele!" ²⁴ Anati kwa iwo, "Ikankhoni nzeru pa zimene mumvela, cifukwa ndimpimo wamene mupimilamo, azasebenzesya mupimo wamene uyo uzapasidwa kwanu. ²⁵ Cifukwa aliwonse amene alinavo, kuli yeve zizapasidwa zambiri, ndi kuli uyo alibe , zizapokedwa cukanga zimene alinazo." ²⁶ Ndipo anati, "Ufumu Pamene wa Mlungu uli ngati munthu amene anafesa mbeu yake pansi. ²⁷ Pamene anagona usiku pamene anauka mmawa, mbeu inayamba kumela ndikukula, cukanga iye sanazibe zimene zinacitika. ²⁸ Nthaka inayamba kubeleka zipatso: poyamba mpunga, pavuli pake mbeu. ²⁹ Pamene inapya mumela nthawi yamene iyo anatuma bavikwakwa, cifukwa nthawi yokolola inafika." ³⁰ Ndipo anati, "Tizayelegeza ndiciyani ufumu wa Mlungu, kapena ndifanizo yabwanji yamene tizasebezesho kukamba? ³¹ uli ngati kambeu kampiru, kapene kanafesedwa, ndikang'ono kwambiri pambeu zonse pa dziko lapansi. ³² Koma pamene kafesedwa, ndikukula kamakala kakulu kupambana cimumtemgo cilicose ca mdimba, ndipo kamankhala ndi misambo zikulu, ndipo mbalame zamumulenga-lenga zimabwela ndikumanga visa mucifule cake." ³³ Ndi mafanizo yambili yotelo anakamba mau kwa iwo, monga mwamene anamvesesa, ³⁴ ndipo sanakambepo ciliconse kosasebenzesha fanizo, koma pamene anali yeka, anafotokoza zonse kwa wophunzila ake. ³⁵ Pa siku ija, pamene kunali mumazulo, anati kwa iwo, "Tiyeni kusidya ina," ³⁶ Ndipo anasiya anthu ambiri, anayenda pamodzi ndi Yesu, cifukwa anali kale muboti. Ndipo maboti yena anali naye. ³⁷ Ndipo cimphepo cikulu cinanyamuka mu boti, ndipo boti inazula kwambiri cifukwa ca mawevu. ³⁸ Koma Yesu iye anali pansi pa boti atagona pa kushoni. Ndipo anamuuusha nati, "Mphunzisi, kodi simusamalila kuti tili kufa?" ³⁹ Ndipo, anauka, ndikuzuzula cimphepo cija nati kucimana, "Mtendele, nkala cete." Ndipo mphepo ija inaleka, ndipo kunali cete. ⁴⁰ Ndipo anabafunsa iwo, "Kodi ndiciyani munacita mantha? Kufikila tsopano mulibe cikhulupirilo?" ⁴¹ Anali ndi mantha yakulu ndipo anati kwa wina ndi mzace, " Nidani uyu, cukanga cimphepo na cimana cimumvelela iye?"

Chapter 5

¹ anabwela ku sidya ina ya chimana, kumuzinda wa Gelasene. ² Ndipo panthawipamene Yesu analikucoka mu Boti, munthu wa vimizimu vyonyansa anabwela kucokela ku manda. ³ Munthu uja anali kunkhala ku manda. Kunalibe munthu aliyense amene anakwanisa kumulesa, cukanga macheni sanakwanise. ⁴ Nthhawi yabili anali kunkhala wovaliliwa ndi womangiwa ndi maceni. Anali kujuba ma cheni. panalibe amene anali ndi mpamvu zomugwila. ⁵ Usiku ndi mzuba anali kukala ku manda ndi kumaphiri, analikulila ndi kuzicekha yeka ndi miyala yakutwa. ⁶ Pamene anaona Yesu kucokela patali, anatamangila kwa iye ndi kugwada ppkwa iye. ⁷ Analira kwambiri nati, "kodi takucimwirani ciyani, Yesu, mwana wa Mlungu wamwamba? Nikupempani mwa Mlungu kuti musaniceneke." ⁸ Cifukwa anali kunena kwa iye, "Tuluka mwa munthu uyu, iwe mizimu yonyansa." ⁹ Ndipo anamufunsa iye, "Zinalako ndiwe ndani? Ndipo anamuyankha nati, "Zina langa ndine Cigulu, cifukwa ndise ambiri." ¹⁰ Anamupempha iye mobwezela-bwezela kuti asavicose mumuzinda. ¹¹ Manje nkhumba zambiri zinali kudya pakaluphiri, ¹² ndipo vinamupempha iye, kuti, "Titumene ku nkhumba; kuti tilowemo." ¹³ Ndipo anavilola; Mizimu yonyansa inacokandikungena mu nkhumba, ndipo zinatukila kuluphiri yopolika kucimana, ndipo nkhumba zokwanila tuwu sauzande zinambila mucimana. ¹⁴ Ndipo aja wodyesa nkhumba zinja zinathaba anayenda ndi kuuza zamene zinacitika kumuzinda ndi malo wozungulila. Ndipo anthu ambiri anayenda kukaonelela zamene zinacitika. ¹⁵ Pamene anafika kwamene kunali Yesu anaona uja mwamuna uja amene anali ndi ziwanda- cikamu ca viwanda - alikhale pansi, atavala, ndipo ali ndi kuganiza bwino, ndipo anacita mantha. ¹⁶ Aja amene anaona zamene zinacitika kuli uja mwamuna amene anali ndi ziwanda anawauza zamene zinacitika kuli iye ndi vyamene zinacitika ku nkhumba. ¹⁷ Ndipo anamupempha kuti acoke kumalo aja. ¹⁸ Ndipo pamene anangena mu boti, uja mwamuna amene ziwanda zinacoka mwa iye anapempha kuti ayende naye. ¹⁹ Koma iye anamukanila, koma iye anati, "Pita kunyumba yako ndi kuanthu ako kawauze zamene Ambuye akucitila iwe, ndicifundo camene akucitila iwe." ²⁰ Iye anapita ndikuyamba kulankhula zinthu zikulu-zikulu zamene Yesu anamucitila iye ku Dekapolisi, ndipo wonse anadabwa. ²¹ Ndipo pamene Yesu anathauka kusidya ina, muboti, anthu ambiri anafika pamene anali iye, pamene anali mumbali mwa cimana. ²² Umodzi wa atsogoleli wa kacisi, woyitiwa Jailosi, anaza kwa iye pamene anamuona, anagwela pamendo pake. ²³ Anamupemphatso ndi mobwezela, nati, "Mwana wanga mkazi alipafupi kufa. Ndikupemphani, kuti mubwele, kuti muzemumusanjike manja anu, kuti apole kuti ankhale ndi moyo." ²⁴ Anayenda naye, ndipo anthu ambiri anamusatila iye ndikumukuza kwambiri. ²⁵ Apo panali mzimai amene anali wocoka magazi kwa zaka twelufu (12). ²⁶ Anavutika kwambiri popita kuvipatala vyosiyana-siyana ndi anasewenzesa ndalama zake zonse, koma sanapole koma matenda anayendelela patsogolo. ²⁷ Pamene anava zimene anthu analikulankhula za Yesu, Iye anabwela ku mbuyo kwake pamene anali kuyenda, anagwila nsoga ya covala cake. ²⁸ Cifukwa anati, "Ngati ndingagwileko cabe covala cake, ndizacilisika." ²⁹ Pamene anamugwila iye, magazi analeka kucoka, ndipo anamvela mutupi mwake kuti acilisika kumatenda aja. ³⁰ Panthawi yamene ija Yesu anazindikila kuti mpamvu zacoka muli iye. Ndipo anayangana kumbuyo kwamene kunali anthu ambiri nafunsa nati, "Ndani wanikuza covala canga?" ³¹ Wophunzila ake anati, "Muona anthu awa ambiri alikukugundani, ndipo inu mulikunena kuti, 'ndani wakugwilani?'" ³² Koma Yesu anayangana kuti amuone wamene anacita izi. ³³ Pamene mzimai, anaona zimene zinamucitikila, anacita mantha ndikuthutuma. Anabwela ndikugwa pansi pafupi ndi iye ndikumuuza coonadi conse pazimene zinacitika. ³⁴ Anati kwa iye, "Mwana wanga mkazi, cikhulupiliro cako cakucilitsa. Pita mumtendele ndipo cilisika ku matenda yako." ³⁵ Pamene anali kulankhula naye, anthu ena anabwela kucokela kunyumba ya uja mtsogoleli wa sunagogi, nati, "mwana wanu mkazi wamwalila. Cifukwa ncani mupitiliza kumuvutisha mphunzitsi?" ³⁶ Koma pamene Yesu anamvako zimene analikulankhula, iye anati kumtsogoleli wa sunagogi, "Usacite mantha. Kuluphilira cabe." ³⁷ Sanavomeze kuti wina ayende naye, koma Petulo, Yakobo ndi Yohana, ndimbale wa Yakobo. ³⁸ Anafika kunyumba kwa uja mtsogoleli ndi anaona anthu ambiri alikumpanga congo; analikulira ndikupunda kwambiri. ³⁹ Pamene anangena munyumba, anati kwa iye, "Cifukwa nicani muli wosweka mitima ndipo muli kulira? uyu mwana sanafe wagona cabe." ⁴⁰ Ndipo iwo anamuseka iye. Koma anawacosa panja ndipo anathenga atate ndi amake amwana ndi aja amene anabwela nawo, ndikupita mwamene munali mwana. ⁴¹ Anathenga zanja la mwana ndipo anati, "Talitha Kumi," kutanthauza kuti, "Mwana wacicepele, ndinena nawe, Uka." ⁴² Panthawi yamene ija mwana uja anauka ndikuyamba kuyenda (cifukwa anali twelufu (12) zaka) ndipo wonse anadabwa. ⁴³ Ndipo anawauza mosimikiza kuti munthu aliyense asaziwe izi. ndipo anawauza kuti amupase mwana uja mkazi kuti ampase zakudya adye.

Chapter 6

¹ Ndipo ancokako kuja ndi kupita kumuzida wake, ndipo wophunzira anamusata iye. ² Pamene sabata inafika anali kuphunzitsa musunagoge. Anthu ambiri anamva ndipo anadabwisika. Anati, "Anacotsa kuti ziphunziso zotele?" "Kodi nzelu izi zamene zinapasidwa kwa iye nizabwanji?" "Nanga izi zodabwitsa zamene iye ali kucita?" ³ "Kodi uyu siuja mpala mathabwa mwana wa Maliya and mkwawo wa Yakobo na Jose na Yudas na Simoni? Nipo alongo ake sali naife pano?" Ndipo anakumudwisiwa ndi Yesu. ⁴ Ndipo Yesu anati kwa iwo, "Mneneli samakhala opanda ulemo, kucosako cabe kumudzi kwake ndipakati ka enekwawo ndi banja yake." ⁵ Analepelakucita zambiri zodabwitsa, kucoselako cabe kusanjika manja yake paodwala ang'ono cabe ndikuwacilisa. ⁶ Kusakhulupirira kwawo kunamudabwisa iye. Ndipo anapita kumidzi yozungulira ndikuphunzitsa. ⁷ Ndipo anaitana aja twelufu (12) ndikuwatuma kuti apite awili - awili, ndipo anawapasa ulamuliro pamizimu yonyansa, ⁸ anawalamulira kuti asanyamule ciliconse paulendo, koma cabe ndodo: asanyamule buledi, kapena thumba, kapena ndalama mucikwama, ⁹ koma avale nkwabilo asavwale minjilo iwili. ¹⁰ Ndipo anawauza kuti, "Pamene mungena munyumba, munkhale mwamene muja kufikila pamene muzacoka malo yaja. ¹¹ Ndipo ngati mumzinda muja sanakulandileni kapena kukumvela inu, pamene mucoka malo aja mukunkhumule doti yakumendo kwanu ngati umboni kwa iwo." ¹² Anapita kukalalikira kuti anthu atembenuke kucoka kuviipa vawo. ¹³ Anacosa ziwanda, ndi kuzoza ndi mafuta odwala ambiri ndipo anawacilitsa. ¹⁴ Mfumu Herode anavela izi, cifukwa zina la Yesu ianamveka pali ponse. Ena anati, "Yohane Mbatizi auka kwa kufa ndipo cifukwa ca ici, zodabwitsa za mpamvu zili kusewenza mwa iye." ¹⁵ Ndipo ena anati, "ndi Eliya." ena anatitso, "Ndi mneneli, ngati uja wa kale." ¹⁶ Koma pamene Herode anamva izi anati, "Yohana wamene ndinadula mutu wauka." ¹⁷ Cifukwa Herode anatuma nthumi kuti Yohana amangiwe ndipo anamangiwa cifukwa ca Herodiya (Mkazi wa mbale wakeFilipo) cifukwa anamkwatila iye. ¹⁸ Cifukwa Yohana anamuza Herode, " Sicinthuncovomelekeza kulti iwe umukwatile mkazi wa mbale wako." ¹⁹ Koma Herodiya iye anakwiya ndikufuna kumupa Yohana, koma analephela, ²⁰ cifukwa Herode anaopa Yohana; anazindikila kuti anali wolunga ndipo woyela, ndipo anazimusunga bwino, kumvwelela iye kunamupanga iye kumvwela kuipa kwambiri, koma anamvwela mokondwela. ²¹ Koma mpata unapezeka pamene Herode anali ndi pwando kusekelela siku yamene anabadwilamo ndipo anapanga cakudya camazulo ca anyanchito wake, ndi akulu asilikali ndi atsogoleli a Galileya. ²² Mwana mkazi wa Herodiya anaza kuzawabvinila, ndipo anakondwelesa Herode ndi alendo woitanidwa. Mfumu inati kukamsikana, "Nipemphe ciliconse camene ufuna nizakupasa." ²³ Analapa kwa iye nati, " Ciliconse camene uzapempha kwa ine, nizakupasa, cukanga pakati ka ufumu wanga," ²⁴ anabwelela kukafunsa amai ake, "Kodi ndikapempehi cyani?" Anati, " Mutu wa Yohane mbatizi," ²⁵ Ndipo anangena mwacangu panthawi yamene ija kwa mfumu, nati, " Ndifuna inu mundipase mwamsanga, pa mbale, mutu wa Yohana mbatizi." ²⁶ Ngakale kuti ici cinakumudwisa mfumu, sanakane kucitha cifukwa analonjeza kudala ndicikwa ca alendo aja amene anaitana. ²⁷ Telo mfumu inatuma asilikali womuyanganila ndi akulu asilikali kuti akamuletele mutu wa Yohana. Ndipo womuyanganila anayenda mundende ndikukajuwa mutu. ²⁸ Anaubwelesa mutu pa mbale ndikuzapasa msikana ndi msikana anapasa amai ake. ²⁹ Ndi wophunzila ake, pamene anamva izi, anabwela ndi kutenga mtembo ndikukaika ku m'manda. ³⁰ Apositolo, anakumana pamodzi ndi Yesu, ndikumuuza iye zamane anacita ndi zamene anaphunzisa. ³¹ Ndipo iye anati kwa iwo, "Bwelani inu noka mupite kumalo kulibe anthu mukaphumuleko kwa kanthawi." Cifukwa ambiri anali kubwela ndikupita, analibe nthawi cukanga yakudya. ³² Ndipo anapita muboti kumalo yopanda anthu. ³³ Koma anawaonandipo ambiri anawazindikila iwo, ndipo anathawa ndi mendo m'muzinda wonse, ndipo anafika koyamba asanafike iwo. ³⁴ Pamene anafika kumbali kwa cimana, anaona cigulu ca anthu ndipo anawacitila cifundo cifukwa anali ngati nkhusa yopanda mbusa. Anayamba kuwaphunzisa zinthu zambiri. ³⁵ Pamene nthawi inasila, wophunzila ake anaza kwaiye nati, "Aya malo niyopanda anthu ndipo nthawi yatha. ³⁶ Muwalole awa anthu apite pafupi m'muzinda ndi m'minzi kuti akaguleko zakudya zawo." ³⁷ Koma iye anawayankha nati kwa iwo, "Imwe muwapase zakudya," Anati kuli iye, "Kodi tingayende kukagula ndi tuu hunderedi denari ya buledi ndi kuwapasa kuti adye?" ³⁸ Iye anati kwa iwo, "Muli ndi buledi ingati? pitani mukaone." Pamene anaona anati, "Buledi mitanda isanu ndi nsomba ziwili." ³⁹ Anawalamulila kuti ankhale mphasi mumagulupu pa uzu wa msipu. ⁴⁰ Ndipo anankhala mumagulupu; magulupu ya mahunderedi (100) ndi mafifte (50). ⁴¹ Anathenga mitanda isanu ya buledi ndi nsomba ziwili, ndipo anayangana kumwamba ndikuyidalitsa ndi kusuna ndikupasa wophunzila ake kuti apase anthu. Ndipo anagawana nsomba zija ziwili kwa wonse. ⁴² ⁴³ ⁴⁴ Ndipo wonse anadya ndi kukutha. Anathenga zosala za buledi, mabasiketi fulu yokwana twelufu, ndi ziduswa za nsomba. Ndipo anali anthu wokwana faivi sauzande amuna amene anadya buledi. ⁴⁵ Panthawi yamene iyo anauza wophunzila ake kuti angene mu boti ndi kupita patsogolo pawo kusidya ina ya cimana, ku Besaida, pamene anauza anthu kuti

abwelelemo kumanyumba yawo. ⁴⁶ Pamene anapita, anakwela kuluphiri kukapemphela. ⁴⁷ Pamene kunali m'mazulo, boti inafika pakati kacimana, ndipo analiyeka kusidya. ⁴⁸ Ndipo anaona kuti walikuvutika ndi cimpepho cifukwa anali kuyenda kosiyana ndi cimpempho cecedwa woyasi. panthawi ya folo koloko usiku anaza kwa iwo alikuyenda pa cimana, ndipo anafuna kuwapitilila. ⁴⁹ Koma pamene anamuona iye ali kuyenda pa cimana, anaganiza kuti nicimzukwa ndipo analira, ⁵⁰ cifukwa anamuona iye ndipo anacita mantha. Panthawi yamene ija analankhula nawo nati kwa iwo, " limbani mtima!, msacite mantha !" Ndine! ⁵¹ Anangena mu boti mwamene munali iwo, ndipo cimpepho cinaleka kuwomba. Ndipo wonse anadabwa. ⁵² cifukwa sanamvesese za mitanda ya buledi zimene ithanthauza, koma mitima yawo inali youma. ⁵³ Pamene anafika kusidya ina yacimana, anafika kumalo wocedwa Genesareti ndipo anaimisa boti. ⁵⁴ Pamene anaseluka mu boti, anamuzindikira iye. ⁵⁵ Ndipo anathamanga m'muzinda ndikuyamba kubwelesa wodwala kwa iye pamamphasa, kwamene anavelela kuti alikupitira. ⁵⁶ Panthawi iliyonse pamene angena m'munzi kapena m'muzinda kapena mudziko, anali kuika wodwala pamalo a msika, ndipo kumphempa kuti nyula yake ayigwireko. Ndipo ambiri amene anaikuza anacilisika.

Chapter 7

¹ Bafalisi na balembe benangu bamene banachokela ku Yelusalemu banasonkhana pamene anali. ² Ndipo anaona kuti wophunzila bake benangu banalikudya buledi na manja yodesedwa, yamene yosasamba. ³ (Chifukwa Bafalisi na Mayuda wonse sibanali kudya wosasamba kumanja, chifukwa banagwililila kumwambo wa makolo. ⁴ Pamene Bafalisi bachokela ku msika, sibanali kudya ngati sibanasambe, na kugwililila ku vinthu vonse vinangu banalandila, monga ku kusuka makapu, mapoto, viya na Tebulo yodyelapo.) ⁵ Bafalisi na balembe banamufunsa Yesu, " Kodi nichani wophunzila bako sibayenda mumwambo wa makolo, chifukwa bakudya buledi wosasamba kumanja?" ⁶ Koma anabauza kuti, "Yesaya ananenela bwino pali imwe bachinyengo. Chinalembewa, 'Aba banthu banilemekeza na milomo chabe, koma mitima ili kutali na ine. ⁷ mapembezo yalibe chilichonse ndiyo banipasa, kuphunzisa malamulo ya banthu monga chipunziso chawo. ⁸ Munataya malamulo ya Mulungu ndikukonkha miyambo ya banthu." ⁹ Anabauzanso kuti, "Munachita bwino bwanji pokana malamulo a Mulungu kuti musunge miyambo yanu! ¹⁰ Chifukwa Mose anakamba kuti, 'Lemekeza batate bako na bamai bako,' Aliyense wamene akamba voyipa pali batate kapena bamai bake azafa zoono. ¹¹ Koma mukamba kuti, ' ngati munthu akuti kuli batate bake kapena bamai bake, 'Iliyonse thandizo yocokela kwa ine ni Kobani, 'kutanthauza kuti, 'yopasiwa kwa Mulungu'- ¹² Ndipo simufunika kumuvomeleza munthu uyo kucita chilichonse kuli batate bake kapena bamai bake. ¹³ mupanga mau ya Mulungu kunkala yalibe mpamvu chifukwa miyambo yanu yamene mupasana. Navinthu volingana vamene muchita." ¹⁴ Anaitana gulu yabanthu na kukamba kuti, " mvelani kwa imwe, imwe bonse, na kumvesesa. ¹⁵ Kulibe chochokela kunja kwa munthu chingaononge munthu pamene chingena mkati. Koma chamene chichokela mukati mwa munthu ndiye chingamuononge." ¹⁶ Yense ali ndi makutu amve ¹⁷ Manje pamene Yesu anachoka pa gulu ya banthu na kungena munyumba, wophunzila bake banamufunsa pali fanizo. ¹⁸ Yesu anakamba kuti, " Naimwe mukalibe kunkala nachinveseso? Simuona kuti chamene chingena mu munthu kuchokela kunja sichingamuipe munthu, ¹⁹ cifukwa siciyenda mkati mwa mtima, koma cimayenda m'mala ndikupita ku ciphuzi?" pali ici Yesu anatanthauza kuti cakudya chili chonse nichoyela. ²⁰ Anakamba kuti, "Ni chija chamene chicokela mukati chamene chiipisa munthu. ²¹ Chifukwa kuchokela mukati mwa munthu, kuchokela mumutima, muchokela maganizo yoipa, zachiwelwele, zaukawalala, zakupaya, ²² zachigololo, zokumbwa, zoipa, zachinyengo, kuzitukumula, zopusa. ²³ Zonse izi zoipa zichokela mukati, ndiye zimene ziipisa munthu." ²⁴ Anaima nakuchoka kuja na kupita kudela ya Tire na Sidoni. Kwamene kuja anayenda munyumba, ndipo sanafune munthu aliwonse kuziba kwamene analili, koma sanakwanise kubisama. ²⁵ Koma pamene mukazi wamene anali na mwana wake mukazi wamene anali na mizimu yonyasa ananvela pali eve, anabwela kuli eve na kugwada pansu pa mendo yake. ²⁶ Mukazi uja anali wa chigiriki, mutundu wa Musurofonika. Anamupempha kuti achose chibanda kuchoka mumwana wake mukazi. ²⁷ Anamuza kuti, "Leka bana badye choyamba. Chifukwa sichili bwino kutenga buledi ya bana na kuponyela bagalu." ²⁸ Koma anayankha na kuli eve, "Zoono, Ambuye, chikanga ibwa zimadyako vamene vikugwa pa tebulo yamene bana badyelapo." ²⁹ Anamuza kuti, " Chifukwa cha vamene wakamba, ndiwe womasuka kuyenda. Vibanda vatuluka mu mwana wako mukazi." ³⁰ Anabwelela kunyumba kwake nakupeza mwana wake muzazi aligone pa mpasa, na vibanda nishi vayenda. ³¹ Ndipo anachoka nafuti kuchoka ku muzinda wa Tire, na kupitilila ku Sidoni ku nyanja ya Galileya kufikila ku malo ya ku Dekapolisi. ³² Ndipo anamuletela munthu winangu wamene sanali kumva ndipo wosalankula, ndipo anamupempha kuti amusanjike manja yake pali eye. ³³ Ndipo anamutenga eve pambali kuchoka pa gulu ya banthu, anaika chikumo cake mumakutu yake, na kutunya mata na kugwila lulime lwake, ³⁴ Analangana kumwamba, nakumuza kuti, "Efefata," kutantauza kuti, "Seguka!" ³⁵ Pantawi yamene iyo matu yanaseguka, ndi camene cinalikugwila lilime lake cinaonongeka ndipo anayamba kulankhula bwino. ³⁶ Ndipo analamulila beve kuti basauze munthu aliyense. Koma mwamene anabauzila maningi, ndiye mwamene banauzila maningi banthu. ³⁷ Banali wodabwa maningi, na kukamba kuti, " Achita vintu vonse bwino. Alengesa na wosanvela kuyamba kunva na wosakamba kuyamba kukamba."

Chapter 8

¹ M'masiku aja, kunalitso anthu ambiri, ndipo analibe cakudya. Yesu anaitana wophunzila ace nati kwa iwo, ² "Nili ndi cifundo ndi anthu awa cifukwa ankhala na ine tsopano kwa masiku yatatu popanda cakudya. ³ Ngati tizawalola kuti apite kumanyumba yawo wopanda kudya, angakomoke munjila. Ena mwaiwo acokela kutali." ⁴ Wophunzila anamuyankha iye, "Kodi ndikuti kwamene tingagule buledi yokwanila wonse kumalo kuno kwamene tilili kopanda anthu kuno?" ⁵ Iye anawafunsa, "Kodi muli ndi mikate ingati?" Iwo anati, "Seveni." ⁶ Anawalamulila wonse anthu kuti ankhale pansi pa msili. Anathenga mitanda ija seveni, nayamika, ndi kuinyema pakati, Anawapasila wophunzila ake kuti awapase anthu, anawapasa anthu. ⁷ Iwo anali ndi tisomba tung'ono ndipo pambuyo poyamika, analamulila wophunzira kuti agawiletsa anthu. ⁸ Anadya ndipo anakutha. Ndipo anatheka nyenswa zosala, mabasiketi yakulu yali seveni. ⁹ Panali anthu wokwanila folo sauzande. Ndipo anawalola tsopano kuti apite. ¹⁰ Panthawi yamene yamene iyo, anangena m'boti ndi wophunzila ake, ndipo anayende ku cigawo ca Damanuta. ¹¹ Pambuyo pake anaza Afalisi ndi kuyamba kususana naye. Anali kumufunsa cizindikilo cocokela ku mwamba pomuyesa iye. ¹² Analankhula yeka m'mtima nati, "Cifukwa nicani mubadwo uyu ulufuna cizindikiro? Zoonadi ndikuuzani, kulibe cizindikiro cizapasidwa ku mubadwo uyu." ¹³ Ndipo anawasiya iwo, anangenatso m'boti, ndi kuyenda kumbali ina ya cimana. ¹⁴ Tsopano wophunzila anaiwala kunyamula buledi. Munali cabe mtanda umozi wa buledi m'boti. ¹⁵ Anawacenjeza iwo ndi kunena kuti, "Nkhalani celu ndipo woyanganila kususana ndi cizamba ca Afalisi ndi cizamba ca Herode." ¹⁶ Wophunzila anayamba kufusana wina ndi mzace, "Kodi ndicifukwa cakuti tilibe buledi." ¹⁷ Yesu anazidikila pali ici ndipo anati kwa iwo, "Kodi nicifukwa ciani muli kulingilila za buledi kuti mulibe? Kodi simunaziwe? Simunamvesese kodi? Kodi mitima yanu yaleka kuziwa?" ¹⁸ Muli nawo menso, Kodi simuona? Muli nawo matu, Kodi simvela? kodi simukumbuka? ¹⁹ Pamene ndinanyema mitanda faivi ndikudyesa anthu faivi sauzande, ndi mabasiketi yangati yamene anazula ndi nyenswa zosala za buledi yamene munathenga?" Anati kwa iye, "Twelufu." ²⁰ Ndipo pamene ndinanyema mitanda seveni kudyesa anthu folo sauzande ndi mabasiketi yangati yamene munathenga?" ²¹ Anati kwa iye, "Seveni." Iye Anati, "Kodi simvesesa?" ²² Anafika ku Besaida. Anthu anbwalesedwa kwa iye, Mwamuna wosapenya anamupempha Yesu kuti amukuze. ²³ Yesu anamugwila uja wosapenya pakwanja, ndi kuyenda naye kuja kwa mudzi. Pamene anamtayila mata yake kumenso ndi kumusanjika manja yake pali iye, anamufunsa iye, "kodi uli kuona?" ²⁴ Anayangana kumwamba, ndipo anati, "Nilikuona anthu ngati mitengo." ²⁵ Anasanjika futi manja ake pa menso pa uja wosapenya, ndipo pamene anasegula menso ake, menso ake anabwelelamo, ndipo anaona zinthu zonse bwino-bwino. ²⁶ Yesu anamuza iye kuti apite kunyumba yake nati, Usangene m'muzinda." ²⁷ Yesu anapita ndi wophunzila ake kumunzi wa Kaisalia Filipi. Panjira pamene anali kupita anafunsa wophunzira ace, "Kodi anthu akamba kuti ine Ndine ndani?" ²⁸ Anamuyankha iye nati, "Yohana mbatizi. Ena akuti, 'Eliya,' ndi ena, 'Umozi wa aneneli.'" ²⁹ Anawafunsa iwo, "Koma inu mukuti Ndine ndani?" Petulo anati kwa iye, "Inu ndinu Kristu." ³⁰ Yesu anawacenjeza kuti asauze wina aliyense za yeve. ³¹ Ndipo anayamba kuwaphunzisa kuti Mwana wa Munthu afunika kusausidwa pa zinthu zambiri, ndipo azakanidwa ndi azikulu ndi akulu ansembe ndi alembi, ndipo azapaiwa, koma pazapita masiku atatu azauka. ³² Analankula izi momveka bwino. Apo Petulo anamtenga iye pambali ndikuyamba kumuzuzula iye. ³³ Koma Yesu anaceuka nayangana wophunzila ake ndipo anamzuzula Petulo nati, "Coka kumbuyo kwanga, Satana! Suuyika malingililo ako pa zinthu za Mulungu, koma pa zinthu za anthu." ³⁴ Ndipo anaitana anthu ambiri pamozi ndi wophunzira ake, anati kwa iwo, "Ngati pali wina amene afuna kunilondola, afunika kuzitana iye mwini, ndikunthenga mtanda wake, ndikunisata. ³⁵ Cifukwa aliyense amene kusunga moyo wake azautaya, ndi yense amene ataya moyo wake cifukwa ca uthenga wanga, azausunga. ³⁶ Kodi cipindula bwanji ku munthu, kuthenga ziko yonse, ndi kutayamoyo wake?" ³⁷ Kodi munthu angacinjane nacani na umoyo wake? ³⁸ Amene azacita nane nsoni ndi mau anga mubadwo uno wacigololo ndi wocimwa, Mwana wa Munthu azacita naye nsoni akayendobwela mu ulemelelo wa Atate ndi Angelo woyela."

Chapter 9

¹ Ndipo anati kwa iwo, "Zoonadi ndinena kwa inu, alipo pano mwainu wamene sazalawapo ifa akalibe kuonapo ufumu wa Mulungu ulikusika mwa mpamvu." ² Patapita cabe masiku sikisi, Yesu anathenga Petulo ndi Yakobo ndi Yohana, kuluphiri, yeka ndi iwo cabe. Ndipo anayaluka pali iwo. ³ Covala cake cinayela ndi kung'anima, kwambiri, cinayela kupambana ciliconse pano pa ziko lapansi. ⁴ Naye Eliya ndi Mose anaonekela kwa iwo, ndipo anali kulankhula ndi Yesu. ⁵ Petulo anayankha ndikunena kwa Yesu, " Rabbi, cili bwino cabe kuli ife kuti tinkhalilile kuno, telo tiyeni timange misasa itatu, imozi ya Mose, ndi imozi ya Eliya." ⁶ (Koma sanaziwe conena cifukwa anali ndi mantha,) ⁷ Makumbi anabwela ndi kuwavinikila iwo. Ndipo mau anacokela mumakumbi, "Uyu ndimwana wanga wokondedwa. Mveleni iye." ⁸ Mozizimuka, pamene anaona- ona, sanaone munthu wina aliyense pafupi ndi iwo, koma Yesu cabe. ⁹ Pamene analikuseluka luphiri, anawalamulila kuti asauze munthu aliyense camene anaona, kufikira pameneMwana wa Munthu atauka kwa kufwa. ¹⁰ Ndipo anasunga ici cinthu kwa iwo cabe, koma analankhulapo pakati pawo cabe, " kuuka kwa kufa" Kutanthauza cana ¹¹ Anamfunsa iye nati, "Cifukwa cana alembi akunena kuti Eliya afunika kubwela coyamba?" ¹² Anati kwa iwo, "Eliya afunika kubwela coyamba kuti aze aze aike m'malo mwake zinthu zonse. Nanga, cifukwa cana kunalembewa kuti Mwana wa Munthu afunika kusausidwa kuzinthu zambiri ndi kumuyesa ngati alibe nchito kawayaya-wayaya? ¹³ Koma ndikuuzani kuti Eliya anabwela, ndipo anamcitila ciliconse camene anafuna, ngani mwamalembo mwamene anenela za iye." ¹⁴ Pamene anabwela kwa wophunzira ake, anaona anthu ambiri alipafupi ndi alembi alikususana nawo. ¹⁵ Koma pamene anamuona iye, anthu wonse anadabwa ndipo anamutamangila iye ndikukampasa moni iye. ¹⁶ Anawafunsa wophunzira ake, "kodi mulikususana ciyani?" ¹⁷ Munthu wina mucigulu ca anthu anayankha nati, " Mphunzisi, ndinabwela naye mwana wanga kwa inu. Ali na cimzimu camene cimamulesa kukamba. ¹⁸ Nthawi zina cimamupaya ndikumugwesa pansi ndi povu kukamwa, ndikusheta menu, ndipo amauma. Ndinapempha wophunzira anu kuti acicose, koma alephela." ¹⁹ Anayankha iwo nati, " Mutundu wosakhulupirila, kodi ndizakhala nau kufikira liti? Kodi ndizakulolani kufikira liti? Muleteni kwa ine." ²⁰ Anamubwelesa munyamata kwa iye. Pamene mzimu unaona Yesu, Panthawi yamene ija unamugwesa pansi ndikumba kukunyuka. M'nyamata anagwa pansi ndi povu kukamwa. ²¹ Yesu anafunsa atate ake, "Kodi ankhalala so kwa zaka zinganti?" Atate ake anayankha, " Kucokela ku umwana wake. ²² Cankhala nthawi zina kumuponyela ku moto kapena ku manzi kufunisisa kuti cimuononge iye. ngati mungakwanishe kumtandiza napapata mucitileni cifundo, mutandizeni." ²³ Yesu anati kwa iye, "Ngati mukwanisha?" Zinthu zonse zitheka kuli wonse amene akhulupirira. ²⁴ Panthawi yamene iyo atate a mwana analira ndi kunena, " Ndikulupirira! Ndithandizeni kusakhulupirira kwanga!" ²⁵ Pamene Yesu anaona anthu ambiri alikuthamangira kwa iwo, anazuzula mizimu yonyansa ndi kuti, "Iwe cimuzimu cosalankhula ndi cosamvela, ndikulamulira, coka muli uyu, ndipo usakabwelenso muli uyu munthu." ²⁶ Cinalira kwambiri ndikumukunyula mnyamata. Mnyamata anaoneka kwati wakomoka, ndipo ambiri anati, "wafa" ²⁷ Koma Yesu anamnyamula pa kwanja ndikumumiririka, ndipo mnyamata anaimirira. ²⁸ Pamene Yesu anangena munyumba, wophunzira ake anamfunsa kumbali nati, "Cifukwa nicani ife sitinakwanishe kucicosa ?" ²⁹ Iye anati kwa iwo, "Ici camutundu wa so sicingacoke cabe koma na Pemphelo." ³⁰ Anacoka malo aja ndi kupitirira Galileya. Sanafune kuti wonse aziwe kwamene analili, ³¹ cifukwa analikuphunzisa wophunzira ake. Anati kwa iwo, "Mwana wa Munthu azapelekedwa mumanja ya anthu, ndipo azamupaya. Akazamupaya, pazapita cabe masiku atatu azaukansa." ³² Koma sanamvesese mau aya, ndipo anali ndi manta kumfunsa iye. ³³ anaza kukapenauni. ndipo paemene anali m'nyumba anawafunsa iwo, "Kodi munali kulankhula cana mnjira?" ³⁴ koma anali cete. Cifukwa anali kususana pakati kawo m'njira kuti wamkulu ni ndani? ³⁵ Anankhala pansi ndikuitana aja twelufu pamozi, ndi kuwauza aja, " Ngati pali wina amene afuna kukhala woyamba, afunika kunkhala wotela pa wonse ndi mtumiki wa wonse." ³⁶ Anathenga kamwana ndikukaika pakati kawo. Anamnyamula pakwanja nati kwa iwo, ³⁷ "Aliyense amene azalandira mwana ngati uyu mzina langa, alandila inenso, ndipo ngati wina alandila ine, sanalandire ine cabe, koma iyenso amene anandituma." ³⁸ Yohane anati kwa iye, "Mphunzisi, tinaona wina alikutulusa ziwanda mzina lanu ndipo tinamulesa iye, cifukwa satisatira ife." ³⁹ Koma Yesu anati, Musawalese iye, cifukwa palibe amene azacita nchito ya mpamvu mzina langa ndi kuyamba kuninyoza pambuyo paka. ⁴⁰ Aliyense amaene satisusa alinase. ⁴¹ Aliyense amene azakupasani kapu ya manzi kuti mumwe cifukwa muli a Kristu, zoonadi ndinena kwa inu, sazathaya mpoto yake. ⁴² ⁴⁴ Aliyense amene azakumudwisa kamozi ka utu tokhulupirira, cizakhala bwino kwake kutenga cimwala cikulu ndikumumangila naco m'mukosi ndikumuponya mcimana. ⁴³ Ngati zanja lako likukumudwisa, ijuwe. Ciliko bwino iwe kunkangena kumoyo wopanda zanja kupambana kukangena kugehena ndi manja awili kumoto wosazima. ⁴⁵ Ngati kwendo kwako kwakukumudwisa, kjuwe. Kulibwino kwako kukangena ku moyo wolemala kupambana kuponyewa ku

gehena ndi mendo ⁴⁶ awili. ⁴⁷ Ngati diso lako yikukumudwisa, icose. kuli bwino kwako kukangena ufumu wa Mulungu ndi diso imozi kupambana kukangena ku gehena ndi menso awili, ⁴⁸ kwamene kuli vikusi vyamene sivikufa, ndi moto suzima. ⁴⁹ Cifukwa aliyense azayesedwa ndi moto. ⁵⁰ Mcele ndiwabwino, koma pamene mcele ukutha kukonda, kodi ungaupange bwanji kuti ukonde nafuti? Nkhalani mcele pakati kanu, ndipo nkhalani m'mtendele wina ndi mzace."

Chapter 10

¹ Yesu anacoka pamalo paja ndi kupita ku ndela ya Yudeya kumalo yopitilila kamana ka Yolodani, ndipo gulu la anthu linazatso kwa iye. Anali kuwaphunzitsatso, wamene unali mwambo wake. ² Ndipo Afalisi anaza kwa iye kuzamuyesa ndikumufunsa, "Kodi ndicololeka mwamuna kulekana ndi mkazi wake?" ³ Iye anayankha, Kodi Mose analamulila ciani?" ⁴ Anati, "Mose analola mwamuna kulemba kalata kolekana ndikumpeleka kwawo." ⁵ "Ici cinali telo cifukwa ca kuuma mitima yanu niye cifukwa cake analembe lamulo yotelo," ⁶ Koma kuyambila poyamba kwacilengedwe, 'Mulungu analenga mwamuna ndi mkazi' ⁷ Pacifukwa ici mwamuna asiye atate ake ndi amai ake ndi kukakangamilana kumkazi wake, ⁸ ndipo awili azakala thupi imozi.' sono salitso awili, koma umozi mtupi. ⁹ Niye cifukwa cake camene Mulungu wa ika pamozi, pasankhale munthu wocipatula." ¹⁰ Ndipo pamene anali m'nyumba, wophunzila anamfunsa iye nafuti pali ici. ¹¹ Anati kwa iwo, "aliwonse amene aleka mkazi wake ndikukwatila wina amcitila cigololo iye. ¹² Ngati anamleka mwamuna wake ndikukakwatiwa ku mwamuna wina, acita cigololo." ¹³ Ndipo anabwelesa tiana kwa iye kuti atukuze iye, koma wophunzila ake anatuzuzula. ¹⁴ Koma pamene Yesu anazindikila ici, anakumdwa nawo ndipo anati kwa iwo, "Tuloleni tiana tize kwa ine, musatulesa, cifukwa ufumu wa Mulungu niwawo awo ngati tiana. ¹⁵ Zoonadi ndikuuzani inu, aliynse amene sazalandila ufumu wa Mulungu ngati kamwana kang'ono sazalowa." ¹⁶ Ndipo anathenga ana m'manja ake ndikutudalisa pamene anatusanjika manja ake pa tiana. ¹⁷ Pamene anayamba ulendo wake, mwamuna wina anamtamangila ndikumgwadila iye, ndikumpempha, "Mphunzisi wabwino, kodi ndicite ciani kuti ningene moyo wosatha?" ¹⁸ Yesu anayankha nati, "Kodi niciani uniitana wabwino? kulibe wabwino, kucosako cabe Mulungu. ¹⁹ Uziwa malamulo: Usapaye, usacite cigololo, usabe, usacite umboni wa boza, usaname, lemekeza atate ndi amai ako." ²⁰ Mwamuna uja anati, "Mphunzisi, zinthu izi nankhala womvelela kucokela pamene ninali m'nyamata," ²¹ Yesu anamuyangana iye ndi kumkonda iye. Anati kwa iye, "cinthu cimodzi camene usoweka. Ufunika kuti ukagulise katundu wako wonse ndipo ndalama ukapase wosauka, ndipo uzakhala ndi cuma ku mwamba. Ndipo ukabwele ndikunikonkha ine." ²² koma cifukwa ca mau aya anawoneka wosakonda nawo ndipo anacokapo wokumudwisiwa, cifukwa anali ndi cuma cambiri. ²³ Yesu anayangana-yangana ndikuuzza wophunzila ake nati, "Onani kukosa kwa iwo wolemela kungena ufumu wa Mulungu." ²⁴ Wophunzila ake anadabwa pa mau aya. Koma Yesu analakulanso kwa iwo nati, "Ana, Nikovuta kungena ufumu wa Mulungu! ²⁵ Ciliko capafupi ngamila kungena pamulomo wa nyeleti, kupambana munthu wolemela kungena ufumu wa Mulungu," ²⁶ Anadabwa kwambiri ndikukambirana wina ndi mzace, "Manje nindani azaphulumuka?" ²⁷ Yesu anawalangana nati, "Kumunthu nicosatheka, koma osati ndi Mulungu. Zinthu zonse ndizotheka ndi Mulungu." ²⁸ Petulo anayamba kukamba naye, " Onani, Tinasiya zonse ndikukukonkhani inu," ²⁹ Yesu anati, " Zoonadi ndikuuzani inu, palibe amene anasiya nyumba, kapena abale kapena alongo ake, kapena amai ake, kapena atate ake, kapena ana ake kapena malo, cifukwa ca ine m'malo mwa uthenga wa bwino, ³⁰ wamene sazalandila mpaso zopitilila pa hunderedi pano paziko lapansi ; ndi mbale ake, ndi mlongo wake, ndi amake, ndi ana, ndi malo ake, ndikunzunzika, ndiziko likuza, moyo wosatha. ³¹ koma ambiri amene aliwoyamba azakhala wosiliza, ndi wosiliza azankhala woyamba." ³² ³³ ³⁴ Anali pa njira, yopita ku Yelusalemu, ndipo Yesu anali patsogolo pawo. Wophunzira ake anadabwa, ndipo aja amene analikukonkha anacita mantha. Ndipo Yesu anaitanatso pambali aja twelufu wophunzila ake ndikuwauza zamene zizacitika posacedwa kwa iye. Onani, tilikuyenda kuYelusalemu, Mwana wa Munthu azapelekedwa kwa akulu ansembe ndi alembi. Azaweluzidwa kuti ifa ndikupelekedwa kwa ³⁵ Yakobo ndi Yohane ana a Zebediya anabwela kwa iye anati, "Mphuzisi, tifuna inu kuti m'tichitire virivotse vamene tizakupemphani." ³⁶ Anakamba kwa iwo anati, Mufuna kuti ine nikucitireni ciani? ³⁷ "Tiloleni kuti tikakhale nayinu muulemelelo wanu, umonzi kuzanjalamanjai ndi wina kulamanzele." ³⁸ Koma Yesu anayankha nati kwa iwo, "Simuziwa camene mukufutsa. kodi mungakwanilitse kumwa mukapu yamene ningamwelele kapena mungalimbikile ubatizo wamene nizabatizidwa nawo?" ³⁹ Anati kwa iye, "Ndife wokhozeke." Yesu anati kwa iye, "Kapu yamene nizamwelamo, muzamwelamo. Ndipo ndiubatizo wamene ndizabatizidwamo. ⁴⁰ Koma nkhanu yonkhala wina kuzanja lamanja wina lamanzele sindine wamene ningasankhe, koma nikwa iwo amene anakonzekelatu." ⁴¹ Pamene ena aja teni wophunzira ake anamvela izi, anakumudwisiwa na Yakobo ndi Yohane. ⁴² Yesu anawaitana pambali ndi kunena kuti, "Mujiwa aja amene wocedwa oweluza a mitundu amawadyakilia iwo, ndi akulu aboma amasewezesa ulamuliro pali iwo. ⁴³ Koma sicizakhala telo pakati kanu. Amene afuna kukhala mkulu pakati kanu afunika kukhala kapolo wa wonse, ⁴⁴ ndipo aliwonse amene afuna kukhala woyamba pakati kanu akhale wanchito wa wonse. ⁴⁵ Cifukwa mwana wa munthu sanabwele kuti amutumikire, koma kuti atumikire, ndikupeleka umoyo wake ngati nsembe ku onse." ⁴⁶ Ndipo anapyamo ku Yeliko. pamene anacoka ku Yeliko ndi wophunzira ake, ndi anthu ambiri, mwana wa Timaulesi, Batulumewo, mpofu yopempha, inakhala panjira. ⁴⁷ Pamene anamva kuti niYesu waku Nazalet, anayambakukuwa nati, "Yesu , mwana wa Davide, nicitire cifundo!" ⁴⁸ Ambiri anazuzula

mpofu ija, muuzeni kuti akhale cete. koma analirisa, "Mwana wa Davide, nicitilecifundo ine!" ⁴⁹ Yesu anaimirira ndikulamulira kuti abwele kwake. Anaitana mpofu ija, nati, "Usacite mantha ! ima! alikukuitana. ⁵⁰ "anataya koti yake, ndikutamanga ndikubwela kwa Yesu. ⁵¹ Ndipo Yesu anayankha iye nati, "Kodi ufuna ine nikucitire ciani?" Mpofu ija inati, "Rabbi, nifuna kulandila menso. ⁵² "Ndipo Yesu anati kwa iye, "Pita. Cikhulupiriro cako cakucilisa." Panthawi yamene ija anayamba kupenyatso, ndipo anamkonkha iye panjira.

Chapter 11

¹ Manje pamene anabwela ku Yelusalemu, anali kufupi ndi Befifagi ndi Betani, paluphiri lwa Oliva, ndipo Yesu anatuma awiri wophunzira ake ² ndipo anAti kwa iwo, "Pitani ku munzi wakumbali ina. Pamene mngena mzapenza kamwana ka bulu kamene wina akalibe kukwelapo. Mkamasule ndikubwela nako kwanga." ³ Ndipo ngati wina azanena kwa inu, 'cifukwa cani mulikucita telo?' Mmuwuze, 'Ambuye akafuna ndipo tizakabwe lesa mwamsanga.'" ⁴ Ndipo anayenda anampeza mwana wa bulu womanga pongenela kunja kwa njira, ndipo anamumangulula. ⁵ Ndipo anthu ena anali imirire panja anati kwa iwo, "kodi mulikucita ciani, kumasula kamwana ka bulu?" ⁶ Anakamba kwa iwo mwamene Yesu anawauzira, ndipo anthu anawalola kuti ayende. ⁷ Aja awiri wophunzira ake anabwelesa kaja kamwana ka bulu kwa Yesu ndipo anaikapo manyula kuti Yesu akwerepo. ⁸ Anthu ambiri anayazinkha nyula zawo mnjira, ndi ena anayanzikha misambo ya vimitengo vyamene anatyola kufumila muminda. ⁹ Aja amene amene anali patsogolo ndi aja amene anali kumbuyo anali fuula nati, "Hosana! Odala ndi iye amene abwela mzina la Ambuye." ¹⁰ Odala ndi uyo ufumu wa wa atate athu Davide wamene ubwela! Hosana mumalo wokwezedwa mwamba!" ¹¹ Ndipo Yesu anangena m'Yelusalemu ndikuyenda m'tempele ndi kukaona zonse zamene zinalimo. Manje, nthawi itapita kale, anacoka kuyenda ku Betaniya ndi aja tewlufu. ¹² Siku yokonkhapo, pamene anacokela ku Betaniya, anamvela njala. ¹³ Ndipo anaona patali cimtengo ca mkuyu cinali na matepo, anayenda pafupi kukaona ngati angapezeka cipatso momwemo. koma pamene anafika pafupi, sanapezamo ciliconse koma matepo, cifukwa sinali nyengo yake. ¹⁴ Analankhula naco, "Palibe amene azadyamo futi cipatso mwaiwe." Ndipo wophunzira ace anamva izi. ¹⁵ Anabwela ku Yelusalemu, ndipo anangena m'tempele ndipo anayamba kucosa aja wogulisa ndi wogula m'tempele. Anagudubula matebulo ya aja wocinja ndalama ndi ponkhala aja wogulisa nkhunda. ¹⁶ Sanalole aliyense kuti anyamule ciliconse kucosa m'tempele kuti ciguliwe. ¹⁷ Anawaphunzitsa nati, "kodi sivinalembedwe, "Nyumba yanga izacedwa nyumba ya mapemphero ya dziko lonse"? Koma inu mayipanga kunkhala nyumba ya Kawalala." ¹⁸ Akulu ansembe ndi alembi anamva zimene analankhula, ndipo anafuna-funa njira yompayilamo. Anali ndi mantha cifukwa annthu wonse anacitha cidwi ndi ciphunzitso cake. ¹⁹ Ndipo nthawi zonse kukafika mazulo, anthu anali kucoka m'muzinda. ²⁰ Pamene analikuyenda m'mawa mwake, anaona uja mtengo wa nkhuyu wauma kucokela ku mizyu. ²¹ Petulo anakumbuka nati, "Rabbi, Onani! Cija cimutengo ca mkhuyu camene munatembelela cauma conse." ²² Yesu anayankha nati, "Nkhalani ndi cikhulupiriro mwa Mulungu. ²³ Zoonadi ndikuwuzani kuti aliyense amene azalankhula ku phiri iyi,' ndipo sakaika m'mtima wake koma akhulupirira kuti zamene walankhula zizacitika, ndiye camene Mulungu azacita. ²⁴ Ndiye cifukwa cake ndilankhula nanu: Ciliconse camene mzapemphelelapo ndi kupempha , khulupirirani kuti mwacilandila, ndipo cizankhala canu. ²⁵ Nthawi zonse pamene muimirira ndi kupemphera, mufunika kukululukira aliyense amene anakucimwilani, kuti Atatet alikumwamba akukululukireni inutso macimo yanu." ²⁶ koma ngati simukhululukira ena , Atate akumwamba sazakupululukirani nainutsu. ²⁷ Anabwelelatso ku Yelusalemu. Pamene Yesu anali kuyenda m'tempele, Akulu ansembe, ndi alembi ndi akulu anaza kwa iye. ²⁸ Anati kwa iye, "Kodi usewenzesha ulamuliro wotani pa ivi vonse? Ndipo ndindani amene anakupatsa ulamuliro wocita ivi? ²⁹ Yesu anati kwa iwo, " Naine ndizakufunsani funso imozi. Ndiuzeni ine ndipo ndizakuwuzani pa ulamuliro wamene ndicitilamo ivi. ³⁰ Kodi ubatizo wa Yohane, unali wocokela kumwamba kapena ku Anthu? Niyankheni." ³¹ Anakhambilana pakati kawo ndikususana nati, "ngati tizati, 'kucokela kumwamba,' iye azati, 'cifukwa nicani simunamkhulupirire?' ³² Koma tikati, 'kufumira ku anthu,...' analikuyopa anthu, cifukwa anthu wonse anzindikira kuti Yohane anali mneneri. ³³ Ndipo anamuyankha Yesu nati, "Sitiziwa." Ndipo Yesu anati kwa, "Nainetso sindizakuuzani pa ulamuliro wamene nicitila izi."

Chapter 12

¹ Ndipo Yesu anayamba kuphunzitsa mumafanizo. Iye anati, "Mdala wina anabyala munda wake wa mpesa, ndipo anaika linga kuzengulusa munda wonse, ndikukumba kuwelengela mpesa. Anamanga nsanja ya olonda ndikuukongoletsa munda kuli aja wolima mpesa. Ndipo anayenda pa ulendo." ² Panthawi yake, anatuma wanchito kuwolima munda kuti akampaseko zipatso zina zamunda. ³ Koma anamtenga iye, ndikumumenya ndi kumbweza kulibe ciliconse. ⁴ Anatumanso wanchito wina, ndipo anamucita vilonda kumutu ndikumvesa nsoni. ⁵ Anatumatso wina, ndipo uyu anamupaya. ndipo ambiri anawacita cimodzi- modzi, kuwamenya ena ndi kupaya ena. ⁶ Panasala cabe umodzi munthu wotuma, amene anali mwana wake wokonedwa. Anali wosiliza wamene anamtuma kwa iwo. Iye anati, "Iye azampasa ulemu." ⁷ Koma aja olima m'munda anati kwa wina ndi mzace, "Uyu ndiye ndiye wopyana wake. Tiyeni, timpaye, ndipo ife tizakhala wopyana." ⁸ Anamugwira ndi kumpaya ndipo anamponyela kuseli kwa munda. ⁹ Manje, ula mwine wa munda, azawacita? Azabwela ndi kuzawaononga aja wolima munda ndi kupasa munda kuli ena. ¹⁰ Kodi musanawerenge m'malembu? 'Uja mwala wamene womanga anaukhana, wakhala wapangondya. ¹¹ Ici cinacokela kwa Ambuye, ndipo ndicodabwisa ku menso kwathu. ¹² Anafuna kumgwira Yesu, koma anacita mantha ndi kuculuka kwa anthu, cifukwa anaziwa kuti analanhkula fanizo iyi kuwasusa iwo. Telo anamusiya ndi kucokapo. ¹³ Ndipo anatumako Afalisi ndi Ahelodiya kuli iye kuti ampeze na mlandu m'makambidwe. ¹⁴ Pamene anabwela, anati kwa iye, "Mphunzisi, tiziwa kuti inu m'makamba kosayopa munthu, ndipo sim'makamba kuti mvese bwino munthu. M'maphunzisa coonzdi conse ca Mulungu. Kodi nicovomelekezeka kano yai mwalamulo kulipira msonkho?" ¹⁵ Koma Yesu anaziwa malingililo yawo ya cinyengo ndipo anati kwa iwo, "Cifukwa niciyani m'funa kundiyesa? Letani kwa ine ndalama niyiwone." ¹⁶ Anabwelesa imozi kwa Yesu. Anati kwa iye, "Kodi pali mutu ndi malemba andani?" Iwo nati, "Kaisayi" ¹⁷ Yesu anati, Pelekani kwa Kaisayi zinthu za Kaisayi ndi kwa Mulungu zinthu za Mulungu." Anadabwa ndi iye. ¹⁸ Ndipo Asaduki, amene anti kulibe kuukha kwa kufa, anabwela kwa iye. Anamufunsa iye, nati, ¹⁹ "Mphunzisi, Mose analemba kwa ise, 'Ngati mkazi wa mbale wako afa ndikusiya mkazi wake kumbuyo, koma sanasyemo ana, mwamuna afunika akwatire mkazi wa mbale, ndikunkhala naye ana a mbale ake.' ²⁰ Kunali abale ake seveni; woyamba anakwatira ndikufa, sanasiyemo ana. ²¹ Waciwili anamkwatira iye ndipo anafa kosasiyamo ana. Ndiwacitatu cimodzi-modzi. ²² Ndiwa seveni sanasiyemo ana. Posiliza pake, uja mwamkazi anamwaliratso. ²³ Paciukitso, pamene azakaukatso, uja mwanakazi azankhala wandani? Cifukwa wonse aja seveni anamkwatirapo." ²⁴ Yesu anati, "Ici sindiye cifukwa cake mulakwisa, Cifukwa simuziwa malembu kapena mpamvu ya Mulungu?" ²⁵ Pamene azauka kwa kufa, Sikuzakhala kukwatira kapena kukwatiliwa, koma azankhala ngati Angelo a kumwamba. ²⁶ Koma nkhanu ya akufa kuti azauka, kodi simunawelenge mbuku ya Mose, pankhani ya cisamba, mwamene Mulungu analankhulila kwa iye ndipo anati, 'Ndine Mulungu wa Abrahamu ndi Mulungu wa Isaki ndi Mulungu wa Yakobo?' ²⁷ Si Mulungu wa akufa, koma wa amoyo. Mulikusokoneza." ²⁸ Umodzi wa alembi anaza ndi kumva zokambilana zawo; anamva kuti Yesu ali kwayankha bwino. Anamfunsa iye, "Kodi lamulo yofunika kwambiri pa wonse ni iti?" ²⁹ Yesu anayankha, "Lamulo yofunika kwambiri ni iyi, 'Mvera Isilayeli, Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndi umodzi. ³⁰ Ufunika kumkonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako, ndi malingaliro yako yonse, ndi mpamvu zako zonse.' ³¹ Ndipo lamulo yaciwiri ndiyo iyi, 'Uzikonda mnansi mwamene uzikondela weka.' Palibe lamulo loposa aya." ³² Ndipo alembi anati, "Mphunzisi, wabwino! mwakamba zoonza kuti Mulungu ndi umodzi, ndipo kulibe wina koposa iye. ³³ Kumkonda iye ndi mtima wonse, ndikumvesa konse, ndi mpamvu zonse, ndi kukonda mnansi wako mwamene uzikondela iwe weka, ici ciposa nsembe yoshoka kano sembe yopeleka." ³⁴ Pamene Yesu anaona kuti wayankha mwa nzelu, iye anati, "Iwe sulikuthali na ufumu wa Mulungu." Patapita izi, palibe wina anamfunsa Yesu mafunso ena. ³⁵ Ndipo Yesu anayankha, pamene anali kuphunzisa mutempele; iye anati, "nanga bwanji alembi anena kuti Kristu ndi mwana wa Davide?" ³⁶ Davide mwine yeka posogozedwa ndi Mzimu Woyela, anati, 'Ambuye anati kwa Ambuye anga, nkhalu ku zanja langa ya manja, kufikira pamene ndizapanga adani ako kunkhala pansu pa mendo ako.' ³⁷ Davide iye anamuitana iye, 'Ambuye' nanga ziteka bwanji kuti Kristu kukhala mwana wa Davide?" Anthu ambiri anamvela iye mwacikondwelelo. ³⁸ Paciphunzitso cake Yesu anati, "Cenjelani ndi alembi, amene amakonda kuyenda mnjira pamene avala minjira itali ndipo amakonda kupasa moni pamsika ³⁹ ndipo amakonda kunkhala m'malo wolemekezeka mu masunagoge m'mapwando amakonda kunkhala malo ya cifumu. ⁴⁰ Ndipo amavutisha manyumba ya azimai wofedwa, ndipo amapemphela pemphelo itali kuti anthu awaone. Awa anthu azalandila cilango cikulu." ⁴¹ Ndipo Yesu anakhala pansu pafupi ndi thumba yopelekelamo zambale; analikuona anthu ali kupeleka ndalama mthumba. Anthu ambiri wolemela analikupeleka ndalama zambiri. ⁴² Koma wosauka wamasiye anabwela ndi tungwinjiri tuwili, tolingana na peni. ⁴³ Ndipo anaitana wophunzira ake nati kwa iwo, "Zoonadi ndikuuzani, uyu mzimai wamasiye wapeleka zambiri kupambana awa wonse apeleka

mthumba iyi. ⁴⁴ Cifukwa wonse apeleka kulingana ndikukuluka kwa cuma cawo. Koma uyu wamasiye , kucokela mkusauka kwake, apeleka zonse zamene anali nazo."

Chapter 13

¹ Pamene Yesu anayenda kuchoka mutempele, umodzi wa wophunzila bake anati kwa iye, "Mphunzisi, wonani myala zabwino na zomanga zabwino!" ² Anamuuzza kuti, "Waziona izi zomangidwa bwino? Palibe mwala uliwonse wamene uzasala pamwamba pa unzake wamene siuzachosewapo." ³ Pamene anankhala paluphiri lwa Oliva kumbali kwa tempele, Petulo, Yakobo, Yohane na Anduleya anamufunsa kumbali, ⁴ "Tiuziyeni, nanga ivi vizachitika liti? Nichani choonesela kuti ivi vinthu vili pafupi nakuchitika?" ⁵ Yesu anayamba kubauza kuti, "Nkhalani chelu kuti wina asakusobeseni." ⁶ Bambili bazabwela muzina yanga nakuti, 'Ndine wamene, 'ndipo azasobesa bambili. ⁷ Koma mukamvela va nkondo na nkhanu za nkondo, musakavutike mutima, ivi vinthu vifunika kuchitika, koma kusila kwa dziko kukalimbe kucitika. ⁸ Chifukwa ziko iza ukila mosusana na ziko, na ufumu uza ukilana mosusana na ufumu. Kuzankhala chogwendeza ziko mumadela yambili, na njala. Ivi ndivo voyamba va kubaba pobala. ⁹ Nkhalani bachelu. Bazakupelekani kuli bakulu bansaka, ndipo muzakamenyewa mumasunagogi. Muzakaimilila kuli bakulu ba boma na mafumu cifukwa cha ine, ngati umboni kuli beve. ¹⁰ Koma uthenga wabwino ufunika kuti ulalikiliwe ku maiko yonse. ¹¹ Pamene bazakakugwilani nakukupelekani, musakachite nkhuwa kuti tizakakamba chani. Chifukwa pantawi ija, vamene muzakakamba vizakapasiwa kuli imwe; simuzankala imwe wokamba, koma Muzimu Woyela. ¹² Mubale azakapeleka mubale munzake ku infa, ndipo tate azakapeleka mwana wake. Na bana bang'ono bazaukila makolo yawo nakufuna kuti bapaiwe. ¹³ Bazakuzondani banthu bambili chifukwa cha zina langa. koma wamene azalimbikila kufikila kuchimalizilo, uja munthu azaphulumusiwa. ¹⁴ Ndipo mukaona zamalodza zosavomelezewa ziimilila pamene sizifunika kuimilila," (lekani bamene baziba kubelenga banvesese) "lekani awo bali ku Yudeya batamangile ku maluphili, ¹⁵ lekani uyo ali pamwamba pamutenge wa nyumba asaseluke kungena munyumba kapena kuti akatenge chili chonse kuchosa munyumba, ¹⁶ ndipo lekani uyo ali mu munda asabwelele kuti athenge chovala chake. ¹⁷ Koma soka kuli baja bamene bali na bana mumala na bamene onyosha bana mumasiku yaja! ¹⁸ Pemphelani kuti visakachitike muthawi ya mphepo. ¹⁹ Chifukwa kuzankhala mazunzo yakulu, yamene yakalibe kuchitikapo kuchoka pachiyambi, pamene Mulungu analenga ziko lapansi, kufikila manje, kulibe, kapena sikuzankhalanso. ²⁰ Kapena Ambuye akachepeseko masiku, kulibe aliyense wamene azaphulumusidwa. Koma chifukwa cha awo wolungama, bamene awo banasankha, azachosako masiku. ²¹ Koma ngati winangu akuuzani kuti, 'Onani uyu ndiye Kristu!' kapena Onani, kuja ndiye kwamene alili! Musakhulupilile. ²² Chifukwa ba Kristu baboza na baneneli baboza, bazaonekela nakuonesa vizindikilo na vodabwisa kuti baname, ngati nikoteka nakuli awo wolungana. ²³ Nkhalani celu! Nakuuzani vonse ivi pamene nthawi ikhaliko. ²⁴ Koma kukasila kusausidwa pamasiku yaja, zuba izasandulika mudima, mwezi suzapelekanso kuwala, ²⁵ nyenyezi zizagwa kucokela kumwamba, ndi mpamvu zamene zili kumwamba zizasung'uzika. ²⁶ Ndipo muzaona Mwana wa Munthu alikubwela mumakumbi ndi mpamvu zikulu na ulemelelo. ²⁷ Ndipo azatuma bangelo bake azasonkhanisa wonse wolungama kuchokela kumbali zonse zili 4, kuchokela kosilila dziko na kosilila kwa thambo. ²⁸ Mphunzilani chiphunziso cha mutengo wa mukuyu. pamene muona misambo iyamba kupukila ndikuyoyosha matepo, muzibe kuti nthawi ya kupya kuli pafupi. ²⁹ Chimozi-mozi pamene muona ivi vichitika, muzibe kuti ali pafupi, pafupi na pakomo. ³⁰ Zoona nikuuzani, uyu mubadwo siuzapita pamene ivi vizachitika. ³¹ Kumwamba na ziko lapansi zizapita, koma mau yanga siuzapita. ³² Koma kulingana za siku kapena nthawi, palibe wamene azaziba, chikanga bangelo kumwamba, kapena Mwana koma Atate. ³³ Nkhalani acelu! Yanganani ndi kupemphela cifukwa simuziwa nthawi yamene iyo. ³⁴ Cilingana ndi munthu amane anayenda paulendo- anasiya nyumba yake ndikuikamo anchito kuti akale woyiyanganila, aliyense ndi nchito yake ndipo analemba na woyangana kuti ankhole m'maso. ³⁵ Cifukwa cake nkhalani ndi celu, cifukwa simuziwa pamene mwine nyumba azabwela; kungankale m'mazulo, kapena pakati kausiku, kapena pamene kombwe alikulila m'mamawa, nangu kuseni. ³⁶ Ngati azabwela movundumukiza, asakakupezani muli mtulo. ³⁷ Camene nili kunena ine kwa inu ndilikunena kwali aliyense: Nkhalani maso!"

Chapter 14

¹ Kunasala cabe masiku yawiri ikalibe kukumana madyelelo ya Pasika ya Buledi ilibe cotupisa. Mkulu wa ansembe ndi alembi anali kuonapo mwamene angamugwirile Yesu ndikumpaya iye. ² Cifukwa anati, "Kosati panthawi ya bwando, kuti pasankhale Ciwawa pakati ka anthu." ³ Pamene Yesu anali ku Betaniya mnyumba ya Simoni wa makathe, pamene anayandikila ku gome, mzimai wina anabwela ndi botolo ya mafuta yonukila, yodula kwambiri, ya nadi yosayanjana ndi mafuta yena. anapwanya botolo ndi kuthenga mafuta ndikumuzola kumutu. ⁴ Koma ena anakalipa. Anayamba kulankhula kuli wina ndi mzace nati, "Kodi maganizo aya yo ononga bwanji?" ⁵ Aya mafuta yonunkhila kwenze bwino kuti agulise pandalama zopitilila fili hundiredi dinali, ndi kupasa wosauka." Ndipo anayamba kumukalipila iye. ⁶ Koma Yesu anati, "Musiyeni mzimai uyu. Cifukwa nicani mufuna kumuvuta uyu? Acita cinthu cabwino kwambimbiri kwa ine. ⁷ Nthawi zonse muzankhala nawo wosauka, ndipo nthawi iliyonse yamene mufuna kuwacitila cabwino muzawacitila, koma simuzakhala naine nthawi zonse. ⁸ Mzimai uyu wacita camene wakwanisha kucita: Wazoza thupi yanga kukonzeka kuikiwa m'manda. ⁹ Zoonadi ndilankhula ndi inu, kulikonse kwamene uthenga wabwino ulalikilidwa kudziko lonse lapansi, camene wacita mzimai uyu, cizalankhulidwa, mokumbukila iye." ¹⁰ Ndipo Yudas Isikaliyoti, umodzi aja twelufu, anacokapo ndikuyenda kwa mkulu wa ansembe kuti ampeleke iye kwa iwo. ¹¹ Pamene mkulu wa ansembe anamva izi, anakondwela kwambiri ndikulonjeza kumpasa ndalama. Anayamba kusakila njila yompelekele kwa iwo. ¹² Siku yoyamba ya buledi yopanda cotupisa, pamene anapeleka nkhusa nsembe ya pasaka, wophunzila ake anti kwa iye, "Mufuna kuti tiyende kuti tikhakonzeka, kuti tidye cakudya ca pasaka?" ¹³ Anatuma awiri wa wophunzira ake ndikunena nawo kuti, "Pitani kumzinda, mzakumana ndi munthu wonyamula mgomo wa manzi. M'mukonkhe iye. ¹⁴ Pamene azangena mnyumba, nainunso mngene ndipo muti kwa mwine nyumba kuti, 'Mphunzisi anti, 'kodi cipinda canga ca alendo niciti kuti tidyelemo pasaka ndi wophunzira anga?" ¹⁵ Iye azakuonesani cipinda cikulu, capamwamba cokonzelatu bwino. Mutikonzekele ife tonse kwamene uko." ¹⁶ Wophunzila aja ananyamuka ndikuyenda kumzinda. Anapeza zonse nga nimwamene analakambira kwa iwo, ndipo anakonza cakudya ca pasaka. ¹⁷ Pamene kunafika m'mazulo, anabwela pamonzi ndi aja twelufu. ¹⁸ pamene anali kuyandikira pa gome yodyelapo, Yesu anati, "Zoonadi ndikuuzani inu, umodzi wa inu azandipeleka kwa dani." ¹⁹ Wonse anacita cisoni, ndipo anati kwa wina ndi mzace anati kwa iye, "mwacoonadi sindine?" ²⁰ Yesu anayankha ndipo anti kwa iwo, "ndi umodzi wa twelufu, wamene ndizatozela naye buledi pamodzi ndi ine mbale. ²¹ Cifukwa Mwana wa Munthu azayenda ngani mwamene malembo anenela za iye. Koma soka kwa uyo munthu wamene azapeleka Mwana wa Munthu! kunali kwabino kwa iye ngati sanabadwe." ²² Pamene anali kudya, Yesu anatenga buledi, anaidalisa, ndikusuna. Anawapasa iwo nati, "Thengani iyi. Iyi ndiye thupi yanga," ²³ Anathengaso kapu, ndikuyamika, ndikwapasa iwo, ndipo wonse anamwamo. ²⁴ Anati kwa iwo, "Aya ndi magari yanga yacipangano, magari yamene yazacoka ya anthu ambiri. ²⁵ Zoonadi ndinena ndi inu, Sindizamwanso kucokela kucipatso ici ca mpesa kufikila ija siku pamene ndizamwa catsopano mufumu wa Mulungu." ²⁶ Pamene anayimba nyimbo, anayenda kuluphiri ya Olive. ²⁷ Yesu anati kwa iwo, "wonse inu mzagwa, cifukwa kunalembedwa, 'ndizamenya mbusa ndipo nkhusa zizamwazika.' ²⁸ Koma pamene ndizaukisidwa kwa kufa, Ndizakayenda patsogolo panu ku Galileya." ²⁹ Petulo anati kwa iye, "Ngakale kuti wonse azagwa, Ine sindizacita izo." ³⁰ Yesu anati kwa iye, "Zoonadi ndinena ndi iwe, usiku wa lero, akalibe kulira kombwe kawiri, uzanikana katatu. ³¹ "Koma Petulo anati, "Ngati nikufa ndizafa ndi inu, Sindizakukanani inu." Wonse analonjeza cimodzi-modzi. ³² Ndipo anabwela kumalo wocedwa Gesemani, ndipo Yesu anati kwa wophunzila ake, "Nkhalani pano pamene ndiyenda kukapemphela." ³³ Anathenga Petulo, Yakobo ndi Yohane ndi iye ndikuyamba kuvutika n'mtima ndimavuto. ³⁴ Iye anati kwa iwo, "Moyo wanga ndiwovutika kwambiri, kufikira pamuyeso wa imfa. Nkhalani pano ndikuona." ³⁵ Yesu anayendako patsogolo pan'gono, ndikugwa pansi, ndikuyamba kupemphela kuti cinali coteka, iyi nthawi ipitirire pali iye. ³⁶ Iye anati, "Abba, Atate, zinthu zonse ndizotheka ndi inu. Cosani kapu iye pali ine. Koma osati mwacifuniro canga koma canu." ³⁷ Anabwelela ndipo anapeza iwo kuti aligone, ndipo anati kwa Petulo, "Simoni, kodi ulikugona? Kodi sungayembekezeka cabe kwa ola imodzi?" ³⁸ Wona ndikupemphela kuti usangene mumayeselo. Mzimu ulikufuna koma thupi ya lema." ³⁹ Anayendatso patsogolo kukapemphela, ndipo anabwezelapo mau amodzi- amodzi. ⁴⁰ Anabwelatso ndipo anawapeza alimtulo, cifukwa menso yawo analema kwambiri kuti analimbe zoomuza iye. ⁴¹ Anabwelatso kacitatu ndipo anati kwa iwo, "Kodi mukaligone ndikupumula? Kwakwana! Nthawi yafika. Wonani! Mwana wa Munthu alikupelekedwa mumanja ya wocimwa. ⁴² Ukani; tiyeni. Wonani, amene alikunimpeleka ali pafupi." ⁴³ Akali kukamba, Yudas umodzi wa aja twelufu, anafika, ndipo anthu ambiri anali ndi iye ndi malupanga ndi mikondo, ndi mkulu wa ansembe, ndi alembi, ndi akulu. ⁴⁴ Manje uja wompeleka anawauza cizindikiro, Kutu, "wamene ndizakising'a, niwamene. M'mukate ndikumsogozela kukamvalila." ⁴⁵ Pamene Yudas anafika, panthawi yamene iyo anabwela kwa Yesu ndipo anati,

"Rabbi! ndikumkising'a." ⁴⁶ Ndipo anamgwira iye ndikuyenda naye. ⁴⁷ Koma umodzi wa iwo amene anaimirira anathenga cipanga ndi kukuwa kwatu kwa kapolo wa mkulu wa ansembe. ⁴⁸ Yesu anati kwa iwo, "kodi mwabwela na vipanga ndi mikondo kwati mwabwela ku gwira kawalala?" ⁴⁹ Pamene ndinali namwe masiku wonse ndipo ndinali kuphunzisa mtempele simunanigwile ine. Koma izi kuti malembo akwanilisike." ⁵⁰ Ndipo aja wonse amene anali ndi Yesu anamsiya ndi kuthawa. ⁵¹ Mnyamata, wovala zovala za kaniki nayenso anamsatira Yesu. Pamene azibambo anamgwira Yesu, ⁵² anasiya covala zake ndikutawa malisece. ⁵³ Anamsogolela Yesu kwa mkulu wansembe. Kwamene kuja anasonkhana naye akulu ansembe, akulu ndi alembi. ⁵⁴ Manje Petulo analikumsata iye patali, patali ngati nyumba ya mkulu wansembe. Anankhala pakati pa asilikali, amene anali kuota moto. ⁵⁵ Manje mkulu wa ansembe ndi bungwe yonse ya Ayuda anali kufuna-funa umboni womususa Yesu kuti ampaye. Koma sanaupeze. ⁵⁶ Cifukwa ambiri anabwela ndi umboni waboza kumunamizila iye, koma cukanga umboni wawo sunagwirizane. ⁵⁷ Ena anabwelesa umboni waboza kumunenela; iwo anati, ⁵⁸ "Tinamvela uyu munthu akunena kuti, 'Ndingagwese tempele iyi ndimanja yanga, ndipo m'masiku yatatu ndingamange ina yosamangika ndi manja.'" ⁵⁹ Cukanga uyu umboni sunagwilizane. ⁶⁰ Akulu ansembe anaimirira ndikumfunsa Yesu, "Kodi suuyankha? Kodi nizabwanji izi zamene akuneneza iwe?" ⁶¹ Koma anali cete sanayankhe ciliconse. Akulu ansembe anafunsatso nati, "Kodi ndiwe Kristu, mwana wodalisa?" ⁶² Yesu anati, "Ndine. ndipo mzakaona Mwana wa Munthu pamene azankhala kuzanja lamanja la mpamvu ndipo alikubwela m'makumbi kucokela kumwamba." ⁶³ Mkulu wansembe anang'amba covala cake ndikunena, " Tikali kufuna umboni wina?" ⁶⁴ Mwazimvelela noka manyozo. kodi mugamula bwanji?" Wonse anamususa nati ayenela kufa. ⁶⁵ Ena anayamba kumtira mata ndikumvala pamenso ndikumenya iye nati kwa iye, "Nenela!" Asilikali anamtenga ndi kumumenya kwambiri. ⁶⁶ Pamene Petulo anali pansi kunyumba ya wansembe, umodzi wanchito mkazi wa Mkulu wansembe anaza kwa iye, ⁶⁷ Anamuona Petulo pamene anaimirira ku moto alikuota, ndipo anamuyangana kwambiri iye. Ndipo anati, "Iwenso unali ndi mnazarene, Yesu." ⁶⁸ Koma iye anakana, nati, " Sindimuiziwa kapena kumvela zamene ulikulankhula iwe." Ndipo anacoka mnyumba ija ya wansembe. ⁶⁹ Koma uja mwannchitho mkazi anamuona iye ndipo anayamba kulankhulanso ndiaja amene anaimirira paja, " Uyu Munthu ndi umodzi wa iwo!" ⁷⁰ Koma iye anakananso. Patapita kanthawi pang'ono aja amene anaimirira naye analikulankhula kwa Petulo nati, " Zoonadi iwe ndiwe umodzi wa iwo, cifukwa naiwenso ndiwe mgalileya." ⁷¹ Koma iye anayamba kuzitembelela ndi kulapa, " Ine uyu munthu sindimuiziwa amene muli kulankhulapo." ⁷² Kombwe analira panthawi yamene iyo kwaciwiri. Ndipo Petulo anakumbuka mau amene Yesu anakambakwa iye, " Kombwe akalibe kulira kawili, iwe uzanikana katatu." Ndipo mtima wake unasweka ndipo analira.

Chapter 15

¹ M'mamawa, mkulu wa ansembe anakumana pamodzi ndi akulu ndi alembi ndi bungwe lonse ya ciyuda. Anamumanga Yesu ndikumpeleka. Anamtwala kwa Pilato. ² Pilato anamfunsa iye nati, "Kodi ndiwe mfumu ya Yuda?" Anamuyankha iye nati, "Mwakamba ndinu." ³ Mkulu wa ansembe anapeleka milandu yambiri kumunenela Yesu. ⁴ Pilato anamfunsatso iye nati, "Suuniyankha? Ona milandu yamene yakukunenela iwe!" ⁵ Koma Yesu sanamuyanike Pilato, ici cinamudabwisa iye. ⁶ Manje panthawi ya pwando, Pilato analikumasula kaidi umodzi wa m'ndende, kaidi wamene wapempha. ⁷ Munali woukila boma m'ndende, ena anali aja amene wopaya anthu, womangiwa m'ndende cifukwa camilandu yawo, m'nali munthu wocedwa Balabbasi. ⁸ Anthu ambiri anabwela kwa Pilato ndikufunsa iye kuti acite zamene zimacitika nthawi zonse. ⁹ Pilato anayankha iwo nati, "Kodi m'funa kuti nikumasulileni mfumu ya Yuda?" ¹⁰ Cifukwa anaziwa kuti mkulu wa ansembe anapeleka Yesu kwa iye mwalufyengo. ¹¹ Koma uja mkulu wa ansembe anakulumiza anthu ambiri kuti akuwe kuti amumasule Balabbasi. ¹² Pilato anayankhatso iwo nati, "Kodi ndicitenji ciyani ndi mfumu ya Yuda?" ¹³ Anakuwatso nati, "Mpacikeni Iye!" ¹⁴ Pilato anati kwa iwo, "Ndi mlandu wabwanji wamene wacita?" Koma anakuwatso mobwezela bwezela, "Mpacikeni Iye!" ¹⁵ Pilato anafuna kukondelesa anthu ambiri, Ndipo anamumasula Balabbasi, Koma anamgwira Yesu ndikumpeleka kuti ampacike. ¹⁶ Asilikali anapeleka kubwalo la milandu (likulu la boma), Ndipo anaitana pamodzi yonse gulu la asilikali. ¹⁷ Anamuvalika nyula ya kaniki Yesu, Ndipo anapanga cisote ca minga ndikumuiika pamutu wace. ¹⁸ Anayamba kumusalutula iye nati, "Tikuonene, mfumu ya Yuda!" ¹⁹ Anamumenya kumutu ndi mikwapu ndikumutira mata iye. Anamgwadira iye momuseting'a kuti ampembeza iye. ²⁰ Pamene anasiliza kumuseting'a, anatenga covala cake cakaniki ndikumveka mwinjira wake, ndipo anapeleka kuti akampacike iye. ²¹ Anamukakamiza wina woyenda m'njira amene anali kucokela kudziko ina kuti anyamule mtanda wa Yesu, munthu uyu zina lake anali Simoni wakukulene atate a Alekizander ndi Rufusi. ²² Asilikali anambwelesa Yesu kumalo wocedwa Gologota (Kutanthauza, "malo ya fupa yakumutu). ²³ Anamupasa iye vinyu yoyavizya na murel, koma sanamwe. ²⁴ Anampacika ndikugawana mwinjira wake poponya mulondola kuti aziwe kuti nindani afunika kutenga gawo iliyonse ya covala pakati ka asilikali. ²⁵ Inali ola ya citatu pamene anampacika iye. ²⁶ Pacikongwani analemba milandu yake kuti, "Mfumu ya aYuda. ²⁷ "Ndi iye anapacikidwa naye akawalala awiri, wina kuzanja lamanja ndi wina kulamanzele. ²⁸ Ndipo mau anakwanilisidwa yonena kuti, ²⁹ Aja anthu wopita m'njira anamunyoza iye, ndi kusunguza mutu nati, "Aha! uzaononga tempele ndi kuimanga mumasiku yatatu, ³⁰ ziphulumuse iwe weka ndipo useluke apo pamtanda!" ³¹ Cimodzi-modzi mkulu wa ansembe anamusing'a iye, pamodzi mdo alembi, ndipo anati, "Unaphulumusa ena, koma iwe sungaziphulumuse iwe weka, ³² lekani tsopano Kristu, mfumu ya Isilayeli, aseluke kucokela pamtanda, kuti tione ndipo tikuluphirire." Ndi aja amene anapacikidwa naye anayamba kumunenela iye. ³³ Pa ola ya sikisi, kunacita mdima dziko yonse kufikira pa ola ya naimi. ³⁴ Pa ola ya naini Yesu analira ndi kulira kukulu nati, "Eloi, Eloi lama sabakatani?" kutanthauza kuti, "Mulungu wanga, Mulungu wanga, Cifukwa nicani mwanisiya neka?" ³⁵ Ena amene analiimilile paja anamva mau ake ndipo anati, "Onani, alikuitana Eliya." ³⁶ Ena anatamanga, ndikutila vinyo kucisankhu, ndikuikako, ndikumpasa iye kuti amwe. Mzibambo anati, Tiyeni tione ngati Eliya azamuselusa pansi." ³⁷ Ndipo Yesu analira ndi kulira kukulu ndikufa. ³⁸ Cinyula ca mtempele cinang' mbika muvigawo viwiri kucokela pamwamba kufikira pansi. ³⁹ Ndi aja a Kenturio amene anaimirila ndi kuyangana Yesu anaona kuti wafa m'njira yamene ija, anati, "Zoonadi uyu munthu anali Mwana wa Mulungu." ⁴⁰ Kunalitso azimai amene anali kuonelelako patali. Pakati kawo panali Maliya Magadalene, Maliya (amake a Yakobo mtonto ndi Yose), ndi Salome. ⁴¹ Pamene anali ku galileya anamkonkha iye ndikumtumikira iye, Azimai ambiri anabwela naye pamo ku Yelusalemu. ⁴² Pamene kunafika m'mazulo, cifukwa inali siku yacikonzekelo, siku yosatila sabata, ⁴³ Yosefe waku arimataya anafika pamenepo. Anali wolemekezeka mu bungwe yawo, amene anali kuyembekeza ufumu wa Mulungu. Anafika mwampamvu kwa Pilato ndikupempha thupi ya Yesu. ⁴⁴ Pilato anadabwa kuti Yesu anafa kale; anaitana akentuliyo ndikuwafunsa ngati Yesu wafa. ⁴⁵ Pamene Pilato anamva kucokela kwa kentuliyo kuti Yesu wafa, anapeleka thupi kwa Yosefe. ⁴⁶ Yosefe anagula nyula. Anamselusa iye pamtanda paja ndikumvunga mnyula zija ndikukamuika manda amene anafokola mcimwala. Ndipo anaikapo pakhome pa manda cimwala cikulu. ⁴⁷ Maliya Magadalene ndi Maliya amake a Yose anaonapo pa malo pamene anamuika Yesu.

Chapter 16

¹ Pamene siku ya Sabata inatha, Maliya Magadalene ndi Maliya amake a Yakobo, ndi Salome anagula mafuta yonukira kuti akazoze thupi ya Yesu. ² M'mamawa pa siku yoyamba ya wiki, anayenda ku manda pamene zuwa linatuluka. ³ Analikulankhula kuwina ndimzace, "Ndani azaticoselapo cimwala pa khomo ya manda?" ⁴ Pamene anayangana kumwamba, anaona kuti cimwala palibe pa khomo ya manda, cifukwa cinali cikulu kwambiri. ⁵ Anangena mkati mwa manda ndipo anaona mnyamata wovala zoyela, analinkhale kuzanja lamanja, ndipo anadabwa. ⁶ Iye anati kwa iwo, "Musacite mantha. Mulikufuna Yesu, waku nazareti, wamene anapacikidwa. Anauka! mulibe muno. Onanipamene anamuika iye. ⁷ Manje pitani, mukauze wophunzira ake ndi Petulo kuti alikuyenda patsogolo panu ku Galileya. Kunja mzamuona iye, Nganimwane anakuuzilani." ⁸ Anayenda ndikuthamanga kucokela ku manda; Anacitha mantha ndi kuthuthuma. Sanakhambe ciliconse kuli aliyense cifukwa anali ndi mantha. ⁹ Pasiku yoyamba ya wiki, athauka, anaonekela coyamba kwa Maliya Magadelena, uja wamene anacosamo viwanda seveni. ¹⁰ Anayenda ndikukhauza iwo amene anali naye, pamene anali kulira ndi kucita maliro. ¹¹ Anamva kuti ali moyo, ndipo waonekela kwa iye, koma sanakhuluphirire. ¹² Ndipo patapita izi, anaonekela mosiyana kuli awiri a iwo, pamene anali kuyenda kudziko ina. ¹³ Anayenda ndi kukauza wophunzira aja ena, koma sanakhuluphirire iwo. ¹⁴ Yesu pambuyo pake anaonekela kwa aja Eleveni pamene anali kuyandikira ku gome, ndipo anawazuzula iwo cifukwa cosakuluphirira ndi kuuma mitima yawo, cifukwa sanakhuluphirire aja amene anamuona atauka. ¹⁵ Anati kwa iwo, "Yendani kudziko lonse la pansi, ndikulalikira uthenga ku zolengedwa zonse. ¹⁶ Iye amene azakhuluphirira ndi kubatizidwa azaphulumusidwa ndi iye amene sazakhuluphirira azakanidwa. ¹⁷ Ndipo zizindikiro izi zizawasatha iwo amene akhuluphirira: Mzina langaazacosa ziwanda. Azalankhula m'malirime yatsopano. ¹⁸ Azathola njoka ndi manja awo ndipo sizawaluma, ndipo pamene azamwa zinthu zowapaya nazo, sazafa. Azasanjika manja awo pa wodwala ndipo wodwala azapola." ¹⁹ Pambuyo polankhula izi Ambuye kuli iwo, anathengedwa kupita kumwamba ndikukakhala kuzanja lamanja ya Mulungu. ²⁰ Wophunzila anacoka ndikuyamba kulalikira kuli konse, ndipo Ambuye anawasewenzesa kuvomelezela mau ake ndi zizindikiro zinali nawo.

Luke

Chapter 1

¹ Ambiri ayeselela kufaka mundandanda, ndikufotokoza pazinthu zamene zinafikilizi kwaise, ² pamene anazipasila kwaise, iwo amene kuchokela pachiyambi anali akamboni amanso mpenya ndi atumiki autenga. ³ Kodi kwainenso chinaoneka chabwino_ pamene anafunisisa mundandanda paza iyi ntano yazinthu zonse kuchokela kuchiyambi- kuti alembe mundandanda paza iwe, oposa kuchenjelesa Theofilas. ⁴ Ichi chinali mwatelo pakuti muzibe chonadi pazinthu zamene iwo anauziwa. ⁵ Munthawi ya masiku ya Helodi mfumu ya ba Yudah, kunali wina opeleka wansembe ndi zina la Zachariya, kuchekela kuchigao cha Abiya.mukazi wake analikochokela pa bana bakazi ba Aaroni,ndizina lake linali Elizabeta. ⁶ Bonse banali olungama pamanso ya Mulungu, ndi kumvelela yonse malamulo ndi mwambo za Mulungu. ⁷ Koma banalibe mwana , chifukwa Elizabeta anali osabala, ndiponso onse abili anali okula mumuzinku paliija nthawi. ⁸ Koma chinabwelo pezeka kuti Zachariya anali pamanso pa Mulungu, kuchita zinchito zake zaopeleka wansembe kulinganiza na ndandanda ya chigao chake. ⁹ Kulinganiza ndi njila yao posankha kuti niuti opeleka wansembe wamene angatumikile, anasankhiwa ndi njuga pongena mutempele ya Mulungu kukashoka nsembe. ¹⁰ Yonse maunjiunji ya banthu yanali kupempela panja paliija nthawi yamene anali kushoka nsembe. ¹¹ Koma mungelo wa Mulungu anaonekela kwa iye ndikuimilila kuzanja la manja laguwa yansembe. ¹² Pamene Zakaliya anamuona anayofyewa ndi kugwela kwa iye. ¹³ Koma mungelo wa Mulungu ananena kwa iye, "Usayofyewe, Zakaliya, chifukwa mapempelo yako yamveka. mukazi wako Elizabeta azakubalila mwana mwamuna. Uzaumitana zina yake Yohane. ¹⁴ Uzankhala na chimwemwe ndi chisangalalo, ndipo ambiri azamwetukila ku badwa kwake. ¹⁵ Azankhala wamukulu pamanso ya Mulungu. Asakamwepo vinyu loko zozazamwa maningi, ndipo azazowedwa ndi muzimu oyela kuchokela mu mimba mwaba maibake. ¹⁶ ¹⁷ Ndi banthu bambiri baku Isilaeli azapindimukila kwa Mulungu.Iye azaenda pasogolo pamanso ya Mulungu mumuzimu ndi mphamvu za Elijah.Azachita izi kuti apindimule mitima ya azitate ku bana bao, pakuti bajabamene sibamvelela baende mu nzelu zaolungama-nolengesa banthu baMulungu kunkhala okonzekela iye." ¹⁸ ¹⁹ ²⁰ Zakaliya ananena kwamungelo, " kuti ningazibe

bwanji izi? popeza ndine mwamuna okakalamba ndi mukazi wanga niokotata maningi." mungelo anayankha ndi kunena kuli iye, "Ndine Gabuliyela, wamene aimilila mumanso pa Mulungu. nenze ninatumiwa kukamba naimwe, kuleta uyu utenga wabwino. Ndiponso, uzankhala chete, ndikukangiwa kukamba, kufikila na siku lamene izi zinthu zi zafikilizika. Ichi nichifukwa chakuti siunakululupile mau yanga, yamene yazafikilizika pa nthawi yokwana." ^{21 22 23} Koma banthu banali kuembekeza Zakaliya. Anali odabwa popeza kuti analikutaya nthawi yambiri mutempele. Ndiponso pamene anachoka, sianakambe ndi bemve. Anazindikila kuti anaona mansompenya pamene anali mutempele. Anapitiliza kualangiza ziziwiso, ndi kunkhala mwakachete. Inabwela yafika nthawi yake yamasiku yosebenza yanasila, Anaenda kunyumba kwake. ^{24 25} Pambuyo yamasiku aya, mukazi wake Elizabeta anamita. Anazipatulako eka pa myezi zisanu. ananena, "Kuti izi ndiye zamene Mulungu anichitila ine pamene ananiyanganila ndi chisomo pakuti, achosepo manyazi paliine kubanthu." ^{26 27 28 29} Mu mwezi wachisanu na kamozi, Mungelo Gabriela enze anatumiwa kuchokela kwa Mulungu kumuzinda wa Galileyo wamene aitanidwa Nazareti, kukobekela namwali kumwamuna otanidwa zina Yosefe. Anali wambali lamunyumba ya Davidi, Ndi zina lanamwali uyu linali Mariya. Anabwela kwa iye ndi kunena, "Mulibwanji, inu odala! Ambuye alinanu." Koma anali osokonezeka kamba ka mau yake ndiku dabwisiwa nakunena ati kodi, kangankhale kaposhedwe ka bwanji. ^{30 31 32 33} Mungelo ananena kuli iye, "Usayope, Mariya, wapeza chisomo na Mulungu. Ona, iwe uzamita mumimba mwako ndikubeleka mwana mwamuna. Uzamuitana zina 'Yesu.' Azankhala wamukulu, ndiponso azaitaniwa mwana waolemekezeka. Ambuye Mulungu azamupasa ufumu wamumubado wa Davidi. Utumiki wake uzankhala pa nyumba ya Jacob muyayaya, ndiponso ufumu wake siuzasila." ^{34 35} Mariya ananena ku mungelo, "Kodi izi zichitika bwanji, popeza kuti sininagonepo na mwamuna?" Mungelo anayankha ndikunena kwa iye, "Muzimu oyela azabwela pali iwe, ndi mphamvu zawakumwamba zizabwela pali iwe. koma oyela wamene azabadwa azaitaniwa mwana wa Mulungu." ^{36 37 38} Ndiponso ona, mubale wako Elizabeta amita mwana mwamuna muunkonte wake. Uyu nimwenzi wachisanu na kamozi, iye wamene anali kuitanidwa osabala. Kulibe chovuta kwa Mulungu. "Mariya ananena, ona" ine ndine mutumiki mukazi wa Mulungu. Lekani chinkhale vameneivo kulinganisa na utenga wanu." Ndiponso mungelo anamusiya. ^{39 40 41} Koma mariya pamasiku yaja anaima mwamusanga ndiponso anenda muziko lamaphiri, mumuzinda wa judeya. Anaenda munyumba ya Zachariya ndi kuposhana na Elizabeta. Koma chinachitika nichakuti pamene Elizabeta anamvela moni wa Mariya, mwana mumimba yake anajumpa, ndiponso Elizabeta anazozedwa ndi mphamvu za Muzimu Oyela. ^{42 43} ^{44 45} Ananyamula ndi liu lake na kukambila pamwamba, Odala ndinu pabakazi, ndiponso zibeleko za mumimba mwanu nizodala. Ndiponso nichifukwa chachani kuti chachitika kwaine kuti amai ba Mulungu wanga kuti angabwele kwaine? Koma onani, pamene liu lakuposha kwanu labwela kumatu yanga, mwana mumimba yanga ajumpa na chimwemwe. Ndiponso niodala wamene akulupilila chifukwa kuzankhala kufilizika kwamau yamene Mulungu anena kwa iye. ^{46 47} Mariya ananena kuti, "Umoyo wanga ulemekezeka ambuye, Ndimuzimu wanga usangalila Mulungu wa mupulumusi wanga." ^{48 49} Koma ayanganila pankhalidwe langa lapanshi ine kapolo wake mukazi. koma onani, kuchela manje mibado zonse zizani itana odala. chifukwa iye wamene aliwa mphamvu achita zazikulu kuli ine, ndi zina lake niloyela. ^{50 51} Chifundo chake chichokela kumibado na mibado kuli aba bamene ayopa iye. Alangiza mphamvu zake ndi zanja lake; ndi kusalanganya iwo amene aliozikweza mumaganizilo ya mitima zao ^{52 53} Anataya mafumukazi kuchoka pa maufumu wao. Ndiponso anakweza iwo apamalo yapansi. Anazozza anjala ndi zinthu za bwino, koma iwo olemela anabatuma manjamaanja. ^{54 55} Apasila tandizo kwa Izilaeli mutumiki wake, monga mukukumbuka chifundo chake (monga mwamene anakambila kuli azitate atu) kuli Abraham ndi mibado zake muyayaya. ^{56 57 58} Mariya anankhala na Elizabeta monga mwezi itatu ndi kubwelela kunyumba kwake. Koma nthawi yobeleka mwana inafika ndiponso anabala mwana mwamuna, Bamene analikunkhala nao ndi achibululu anamvela kuti Mulungu analangiza chifundo kwa iye, ndiponso anasangalala ndi iye. ^{59 60 61} Koma chinachitika pasiku lachisanu natutatu pamene anabwela kuzembulula mwana. Asembe bamuitana "Zakaliya," zina yaba tate bake, Koma amaibake banayankha ndikunena, "Iyayi azaitaniwa Yoani." Ananena kwaiye, "Ati kulibe paachibululu anu amene ataniwa Yoani." ^{62 63} Anapanga ziziwisilo kwa atate bake kuti azibe vamene enzofuna kumuitana. Atate bake anafunsa tebulo yolembelapo, ndi kulemba, "kuti zina lake ni Yoani." Onse anankhala odabwisiwa pali ichi. ^{64 65 66} Pameneapo chabe kamwakake kana seguliwa ndi lilime inamasuliwa. Anakamba ndiku tamanda Mulungu. Kuofewa kunabwela palionse amene analikungala omuzingulila. Izi zonse zinthu zinawanda monsemonse mumaphiri ya mumuzinda wa judeya. Ndi onse anamvela anazisunga mumitima zao nakunena, "Kodi azankhala mwana wabwanji uyu?" chifukwa zanja la Mulungu ilipali iye. ^{67 68} Batate bake a Zakaliya anazozedwa ndimuzimu oyela ndikupasa uneneli, kuti, Matamando yankhale kuliambuye, Mulungu wa Izilaeli, chifukwa abwela kutandiza ndiponso kufikiliza chiombolo chabanthu bake. ^{69 70 71} Akweza lisengo lakalachipulumuso kuli ise ba munyumba ya mutumiki wake Davidi, monga mwamene ananenela ndi kamwa kaaneneli oyela amene analiko nthawi yakudala. Azaleta chipulumuso kwaadani bathu ndiponso ndi kuzanja yabonse bamene batizonda. ^{72 73 74 75} Azachita izi kuonesa

chifundo kuli azitatate bathu ndiponso kuakumbusa chipangano choyela, chilapo chamene ananena kuli Atate watu Abraham. Analapa kutipasa ise, popeza kuti anatiombola kuchoka kuzanja la badani bathu, kuti tikamutumikile kopanda mantha, muchiyelo na muchilungamo kwaiye masiku yatu yonse.^{76 77} Inde, ndi iwe, mwana, uzaitaniwa muneneli wauyo wapa mwamba, chikufukwa uzaenda pasogolo pamanso yambuye kukonza njila zake, nakukonzeka banthu pakubwela kwake, na kupasa nzelu zachipulumuso kubanhu bake naku kululukila machimo.^{78 79} Izi zizachitika kamba kachifundo cha Mulungu watu, chifukwa chakuti zuba iwala kuchaka kumwamba azabwela kutitandiza, kuwala kuliabo bamene bankhala mumudima ndiponso muchinfwile cha infa. Azachita izi kusogolela mendo yatu munjila ya mtendere."⁸⁰ Koma uyu mwana anakula ndiponso anabwela alimba mumuzimu, ndiponso anali muchipululu kufika namasiku yoonekela potuba kuli a Izilaeli.

Chapter 2

¹ Koma muli yaja masiku, chinabwela chachitika kuti Siza Ogastasi anatuma mbiri yakuti kupenda kwa banthu bonse kuchitike muli ziko lija. ² Ukukunali kupenda koyamba pamene Kilinas anali mukulu waboma mu silia. ³ Koma aliyense anapita kumizinda yao ndi kukalembesa mazina yao. ⁴ Ndi Yosefe anapita kuchokela kugalileyo, mumuzinda wa nazareti, nakuyenda ku judeya, mumuzinda wamene uitanidwa Davidi wamu betilehemu, chifukwa analikuchokela mubanja ya mubado wa Davidi. ⁵ Anapita kuja kukalembesa pamozi ndi Mariya, wamene enze okolobekelwa kuli iye ndiponso anali namimba. ⁶ Manje chinabwela chachitika kuti pamene bakalikwamenekuja, nthawi inafika yobala. ⁷ Anabala mwana mwamuna, mwana wake oyamba, ndiponso anamu vininkila na nyula yopitamo milaini, ndiponso nakumufaka mukola, chifukwa kunalibe malo muja mwamene anafikila. ⁸ Kunali boyembela ngo'mbe muja muchigao bamene banalikunkhala muminda, kuyembela ngo'mbe zao usiku. ⁹ Mungelo wa Mulungu anaonekela kwa iwo, ndi ulrmelelo wa Mulungu unalangisiwa kuli bemve, ndiponso anayofedwa. ¹⁰ Koma mungelo ananena kwa iwo, "musayofedwe, chifukwa naleta utenga wa bwino wamene uzabwelesa chimwemwe chachikulu kubanthu bonse. ¹¹ Lelo mupulumusi abadwa mumuzinda wa Davidi! iye ndiye kilisitu ambuye! ¹² Ichi chizankhala chizibiso chamene chiza pasiwa kuli iwe, uzapeza mwana opombewa munyula yamilaini wamene alimukola." ¹³ Mosachedwa angelo analikwamene kuja nagulu likulu la asikali ochekala kumwamba atamanda Mulungu, ndi kunena, ¹⁴ Ulemelelo kwa Mulungu mumwambamo, ndiponso lekani pankhale mtendere pa ziko kulibaja banthu baja bamene iyo bamvesedwa bwino." ¹⁵ Chinabwela chachitika kuti pamene angelo anachoka pamalo yao ndi kuyenda kumwamba, oyembela ngo'mbe anazi uza iwo oka, "Tiyeni manje ku batilehemu, tikaone ichi chamene chachitika, chamene amuye alengesa kuti ise tizibe." ¹⁶ Anaendisa kuyenda ndiponso anapeza Mariya ndi Yosefe, nakupeza mwana agona mukola. ¹⁷ Pohekala kumuona, analengesa kuziba chamene chinauziwa kuli bemve pamwana uyu. ¹⁸ Bonse bamene bana mvela banali odabwisiwa ndichamene anauziwa nabaja oyembela. ¹⁹ Koma Mariya anangopitiliza kuganizila pazinthu zonse zamene anamvela, ndi kuzisungilila mumutima wake. ²⁰ Oyembela anabwelamo, ndiponso analikulemekeza ndi kutamanda Mulungu palizonse zamene banamvela ndi kuona, monga mwamene chinakambidwa kuli benve. ²¹ Pamene masiku asanu ndi yatatu anafika, ndiyepamene anajubiwa, anaitaniwa zina Yesu, Zina yamene anapasiwa na angelo pamene akalibe kumitiwa mumimba. ²² Pamene masiku ofunikila kuzembululiwa yanakwana, kulinganiza ndi malamulo ya Mosesi, Yosefe ndi Mariya anamuleta mutempele mujelusalemu kumupasila kuli Mulungu. ²³ Monga mwamene chinalembewa mumalamulo ya Mulungu, Mwamuna aliyense wamene amasegula, azankhala opatulidwa na Mulungu." ²⁴ Koma anapeleka nsembe kulinganisa namwamene chinakambiwa mumalamulo ya Mulungu, "Tunkhunda tubili loko tubana tun'gono tubili twamapijoni." ²⁵ Kunaliko mwamuna mujelusalemu otanidwa simoni ndiponso anali olungama ndi ozipelaka. Anali kuyanganila pakubwezewa kwa Izilaeli, ndiponso muzimu oyela anali paliye. ²⁶ Chenze chinavumbulusiwa kwaiye na muzimu oyela kuti siazaona infa pamene akalibe kuona ambuye wa kristhu. ²⁷ Kusogolelewa mwa muzimu, simoni anabwela mutempele. pamene makolo analeta mwana mun'gono Yesu, kubwela kuchita kulinganiza na mwambo wa malamulo, ²⁸ anamutenga mumanja yake ndi kutamanda Mulungu na kunena, " ²⁹ kuti lekani mutumiki wanu ayende mwa mtendere, Ambuye, kulinganiza na mau yanu. ³⁰ Menso yanga yaona chipulumuso chanu, ³¹ chamene mwakonzeka pamanso yabanthu bonse: ³² Nyali yachivumbuluso kuli majenta ndiponso ulemelelo kubanthu banu Izilaeli." ³³ Batate ba mwana na bamai bake anali odabwisiwa panzithu zamene zina kambika pali iye. ³⁴ Simoni anaba dalitsa ndi kune kwa kuli Maliya mai wake, "Onani, uyu mwana anasankidwa kwaio bamene ogwesewa ndi kunyamuliwa kwa banthu bambili mu Izilaeli ndiponso kwachiziwiso chamene chinakaniwa" ³⁵ ndiponso monga lupanga ong'amba umoyo wanu pakuti maganizilo yamitima zambili ya vumbulusiwe." ³⁶ Muneneli otanidwa zina Anna analiko. analimwana mukazi wa faniwelo kuchoka mumutundu wa Asha. Anali mukulu maningi. Anankhala na mwamuna wake zaka makumi ndi awiri kuchokela kuunamwali wake, ³⁷ ndiponso anali ofelewa zaka 80. Sianachokepo mutempele chifukwa analikutumikila mumapempelo ndi kusala kudya, usiku ndi muzuba. ³⁸ pali ijanthawi, anabwela kulibemve ndiponso anayamba kupeleka matamando kwa Mulungu ndi kukamba pa mwana kwa alionse analiku kuembekezela chipulumuso cha Yelusalemu. ³⁹ Pamene anasiliza zonse izi banali kufunikila kuchita kulingani ndi malamulo ya Mulungu, Banabwelela kugalileyo, mumuzinda wao wa Nazareti. ⁴⁰ Mwana anakula ndiponso anali ndi mphamvu, kuchulukila munzeli ndiponso chisomo cha Mulungu chinali pali iye. ⁴¹ Makolo bake banalikuyenda chaka chilichonse ku Yelusalemu kumadyelelo ya paskha. ⁴² Pamene anali ndi zaka makumi yabili ndi tubili, banaendanso panthawi ya mwambo wa madyelelo. ⁴³ Kuchekela pamene banankhalako masiku yokwana yamadyelelo, anayamba kubwelelamo ku nyumba kwao. Koma munyamata Yesu anasalila mu Yelusalema ndiponso makolo yake sibanazibe. ⁴⁴ Banalikuganizila kuti kapena alinagulu yamene anali nao

pamodzi, koma anaenda ulendo uyu siku limozi. Ndiponso anayamba kumusakila kuliba banja lao ndi pa abwenzi ao. ⁴⁵ Pamene sibana mupeze, anabwelela ku Yelusalemu ndi kuyamba kumu sakila kuja. ⁴⁶ China bwela chachitika kuti pochokakela masiku yatatu, Bana mupeza mutempele, Enze nkhezi pakati ka apunzisi, kumvelela kwaiwo ndi kufunsa mafunso. ⁴⁷ Bonse banamumvela anadabwa pa kumvesesa kwake ndi mayankho yake. ⁴⁸ Pamene bana muona, bana dabwa. bamai bake bananena kuli iye, "Iwe mwana, nichifukwa chachani watichitila ivi iyi njila? Mvela ine nabatate bako tenzekukusakila." ⁴⁹ Ananena kwaiwo, Nichani chamene munisakilila? kodi simunazibe kuti nifunikila kupezeka munyumba ya batate banga?" ⁵⁰ koma sibanamvesese chamene analikutanthauza pa mau aya. ⁵¹ Ndipo anabwelela kunyumba ndi benve ku Nazaleti ndiponso anali omvelela kwa iwo. Bamai bake anasungilila zonse izi mumutima wao. ⁵² Koma Yesu anapitiliza kukula munzeli za kuya ndi kutupi, ndiponso anachulukila muchisomo na Mulungu ndipo ku banthu.

Chapter 3

¹ Muchaka chakumi ndi tusanu pamene analikulumulila Tibarias siza_ pamene ponshas pailleti anali mukulu wa boma mu judeya, Helodi anali tetrachi wamu galili, mubale wake philipu anali tetrachi muchigao cha ituriya ndiponso trachonitis, ndiponso lysanias anali tetrachi wa Abileni, ² ija nthawi ya opeleka nsembe ya Annas ndiponso kefasi_ mau ya Mulungu wanabwela kuli Yoani mwana wa Zakaliya, muchipululu. ³ Anaenda muchigao chozungulila Jodani, kutumikila ubatizi olapa pa kukululukila kwa machimo. ⁴ Monga vamene chinalembedwa mubuku ya mao ndi Yesaya muneneli, "Liu laumozi lilikuitana muchipululu, 'Konzekani njila ya Mulungu, konzani njila yake iyondoloke. ⁵ Chipululu chilichonse chizazozedwa, ndiponso phiri ili yonse izabwelesewa panshi, ndiponso njila iliyonse yosayondoloka iza konzewa ndi kuyondoloka, ndiponso ndi ijayosakonzwa iza mangiwamo manjila, ⁶ nkanda yonse izaona chipulumuso chamulungu." ⁷ Ndipo Yoani ananena ku magulu yakulu yabanthu bamene banali kubwela kubadizika ndi iye, " imwe bana banjoka!nindani ukuchenjezani kuti mutabe kuukali wamene ubwela? ⁸ Pokapo, belekani zipaso zamene zoyenekela ndi chilapilo, ndiponso musayambe kunena mwaimwe mweka, ' Kutu tilindi Abraham wamene alinitate watu; ninakuuzani kuti Mulungu akwanisa kunyamulamo bana ba Abraham mumwala izi. ⁹ Apamanje ndi katemo nikokonzeka kuchaya kumizhu zamitengo. koma mutengo ulionse wamene siupeleka zipaso zabwino uzajubiwa pansu ndiponso uzataiwa mumulilo. ¹⁰ Ndipo aya magulu yanapitiliza kumufunsa, ndikunene, "Kuti kansi tingachite bwanji?" ¹¹ Iye anabayanka, ndi kunena kuli iwo, ngati winawache alina na zovala zibili, afunika kugabana ndi mumunthu wamene alibe, ndi uja alina zakudya afunikila kuchita chimozi. ¹² Baja otenga misonko ndi iwo anabwela kubadizika, ndiponso ananena kwa iye, "Mupunzisi, nichani chamene tingachite?" ¹³ Ananena kwaiwo, "Musatenge ndalama zopitilila kupambana pazamene mwauziwa kutenga." ¹⁴ Basilikali ndiwo anamufunsa, ndikunena, "Nanga ise? Tizachita bwanji?" Ananena kwaiwo, Musatenge ndalama kumunthu aliyense mokankamizila, ndiponso musakankamize kunamiza wina mopatikiza.Munkale okutula ndizamene mufola." ¹⁵ Koma pamene banthu banali ndi chilakolako kuembekeza kubwela kwa kristhu, aliyense anali kuzifufuza mumitima mwao paza Yoani ngati angankale kristhu. ¹⁶ Yoani anabayankha bonse, " koma ine, nikubadizani ndi manzi, koma alikubwela winawake wamene alina mphamvu kupambana ine, ndiponso siniyenela ndi kumasula ntambo zansapato zake.Azakubadizani ndi muzimu oyela ndiponso ndi mulilo. ¹⁷ Ndi chokololelako alinacho mumanja kuti awamise bwino gome yake ndiponso kukolola witi kufaka munyumba yosungilamo.koma azashoka zinyalala ndi mulilo wamene siusila." ¹⁸ Ndi bambiri enanso ozinyamula, Yoani analalikila utenga wabwino kubanthu. ¹⁹ Pamene Herodi ndi tetrachi bana vomekezedwa kukwatila mukazi wamubale wao, Helodias, ndi zinthu zonse zonyansa zamene anachita ndi Helod, ²⁰ anafakilako pamilandu zonse zamene anachita: anakomela Yoani mujele. ²¹ Manje chinabwela chachitika kuti, pamene bonse banthu anabadizika, Ndi Yesu anabadizika. Ndiponso pamene akali kupempela, kumwamba kunaseguka, ²² ndi Muzimo Oyela anabwela pansu muchifanikizo chatupi monga nkunda, ndiponso liu linabwela kuchoka kumwamba, " Ndikuti iwe ndiwe mwana wanga mwamuna, wamene nikonda. Ndine okondwela ndi iwe." ²³ Pamene Yesu anayamba utumiki wake, Anali ndi zaka makumi yatatu.Anali mwana mwamuna(wamene benzoganila) kuti ni wa Yosefe, mwana wa Heli, mwana ²⁴ mwamuna wa matthat, mwana mwamuna wa Levi, mwana mwamuna wa Melchi, mwana mwamuna wa Janani, mwana mwamuna wa Yosefe. ²⁵ Yosefe anali mwana mwamuna wa Mattatiyas,mwana mwamuna wa Amos, mwana mwamuna wa Naham, mwana mwamuna wa Esili, mwana mwamuna wa Naagi, mwana mwamuna wa ²⁶ Maati, mwana mwamuna wa Mattatiyas, mwana mwamuna wa Simeni, mwana mwamuna wa Yoseki, mwana mwamuna wa Yoda. ²⁷ Yoda anali mwana mwamuna wa Yoanani, mwana mwamuna wa Resa,mwana mwamuna wa Zelubabel, mwana mwamuna wa Salathio, mwana mwamuna wa Neri, ²⁸ mwana mwamuna wa Melchi, mwana mwamuna wa Addi, mwana mwamuna wa Kosamu, mwana mwamuna wa Elimadam, mwana mwamuna wa Er, ²⁹ mwana mwamuna wa Yoshua, mwana mwamuna wa Elyaza, mwana mwamuna wa Yorimu, mwana mwamuna wa Matthat, mwana mwamuna wa Levi. ³⁰ Levi anali mwana mwamuna wa Simoni, mwana mwamuna wa Yuda, mwana mwamuna wa Yosefe, mwana mwamuna wa Yonam, mwana ,mwamuna wa Eliakimu, ³¹ mwana mwamuna wa melea, mwana mwamuna wa Menn, mwana mwamuna wa Mattatha, mwana mwamuna wa Nathan, mwana mwamuna wa Davidi, ³² mwana mwamuna wa Yesse, mwana mwamuna wa Obed, mwana mwamuna wa Boazi, mwana mwamuna wa salmoni, mwana mwamuna wa Nahashoni. ³³ Nahashoni anali mwana mwamuna wa Aminadabu, mwana mwamuna wa Adimini, mwana mwamuna wa Arni, mwana mwamuna wa Heziron, mwana mwamuna wa Perezi, mwana mwamuna wa Yuda, ³⁴ mwana mwamuna wa Yakobo, mwana mwamuna wa Isaaki ,mwana mwamuna wa Abraham, mwana mwamuna wa Tera, mwana mwamuna wa Naha, ³⁵ mwana mwamuna wa serugi, mwana mwamuna wa Reu, mwana mwamuna wa Pelegi, mwana mwamuna wa Eba, mwana mwamuna wa Shelah. ³⁶ Shelah anali mwana

mwamuna wa Kanani, mwana mwamuna wa Arphaxad, mwana mwamuna wa Shem, mwana mwamuna wa Noah, mwana mwamuna wa Lameki, ³⁷ mwana mwamuna wa Methusela, mwana mwamuna wa Enoki, mwana mwamuna wa Yared, mwana mwamuna wa Mahalaleel, mwana mwamuna wa Kenani, ³⁸ mwana mwamuna wa Enosi, mwana mwamuna wa Sethi, mwana mwamuna wa Adam, mwana mwamuna wa Mulungu.

Chapter 4

¹ Koma Yesu, kunkhala ozozedwa ndi muzimu oyela, Anabwelela ku musinje wa Yodan, Ndiponso nasogoledwa ndi muzimu oyela kuyenda muchipululu ² mwamene anaenda masiku makumi ndi anai kuyesedwa ndi satana. Sianadye chilichonse masiku yaja, Ndiponso pokusila kwanthawi ija anamvela njala. ³ Satana ananena kwaiye, "Ngati ndiwe mwana wa Mulungu, Sandula mwala izi kunkhala Mukate." ⁴ Yesu anamuyankha, "Nicholembedwa, " Kuti munthu siazankhalila mukate weka." ⁵ Koma satana anamusogolela Yesu kumupeleka pamalo yapamwamba ndiponso anamulangiza maufumu yapaziko pakanthawi kang'ono. ⁶ Ndi satana ananena kwaiye, "Kuti nizakupasa mphamvu zonse ndi ulemelelo, chifukwa wapasiwa kuli ine, ndiponso ningapase aliynse. ⁷ Chifukwa chaichi, ngati unganigwadile pansi ndiponso unipempeze ine, chisankhala chako. ⁸ Koma Yesu anayanka naku kamba kuti, "nicholembewa, 'Upembeze Ambuye Mulungu wako, ndiye wamene eve eka uzatumikila.'" ⁹ Komanso satana anasogolela Yesu ku Yelusalemu nakumupeleka pamalo yotalimpisa yapa tempele, Ndiponso ananena kwaiye, "Ngati ndiwe mwana wa Mulungu zitaye weka pansi kuchokela pano. ¹⁰ Chifukwa chinalembedwa, 'Azatuma angelo abo ameneazakusamalila, ndi kukuchingiliza iwe,' ¹¹ 'Ndiponso, 'Bazakunyamula mumanja yao nakukunyamula pamwamba, kuti usazigwesele pamwala.'" ¹² Napakumuyankha, Yesu ananena, "Chinanenewa, " Kuti usafake Mulungu wako mumayeso." ¹³ Pamene satana anasiliza kumuyesa Yesu, Anamusiya iye ndikuyenda paka panthawi ina. ¹⁴ Koma Yesu anabwelela ku Galili mumphamvu zamuzimu. ndiponso utenga pali Iye unamwazikana malo yonse yenzo zingulila chija chigao. ¹⁵ Ndiponso anayamba kupunzisa mutempele ndiponso bonse anamutamanda. ¹⁶ Iye anabwela ku Nazareti, muzinda mwamene anakulila, ndiponso kulinganiza na mwambo wake, Enze kungena mutempele pasiku la sabata, kulingana ndi mwambo, Ndiponso enze kuimilila ndi kubelenga naliwu lapamawmba. ¹⁷ Buku ya muneneli Aizaya Inapasidwa kuli Iye. Analikusegula buku ija, Ndiponso anapeaza pamalo pamene chinalembedwa, ¹⁸ "Muzimu wa Mulungu alipali ine, chifukwa anizozza ine kulalika utenga wa bwino kuosauka. Anituma ine kulalikila pa kumasusila omangidwa, ndiponso kubwezedwa kwa manso osapenya, ndi kumasula ogwedezeke, ¹⁹ ndi kunenela pachaka za chisomo cha Mulungu." ²⁰ Komanso anaivala buku ija, ndikubwezela bamene analikusunga ndi kunkhala pansi. Manso yabonse muja mutempele yanalipaliche pali enve. ²¹ Anayamba kukamba kuli iwo, "Kuti lelo ayamalemba yafikilizika mukumvela kwanu." ²² Bonse muja mumalo anapelekelala umboni pazamena ananena ndiponso bonse banadabwisiwa pamau yachisomo yamene yanalikuchoka mukamwa kake. Banali kunena kuti, "Uyu ni mwana wa Yosefe, kodi sichochi?" ²³ Ananena kwa iwo, "Chachendi muzanena proverb iyi kuli ine, "Adotolo, zichiliseni mwaka. Vilivonse vamene tinamvela mulikuchita mu kapenamu, chitani chimozi mozi muno mumuzinda wanu." ²⁴ Koma ananena, "Chonadi ninena kwainu, kulibe muneneli wamene analandilidwa mumuzinda wake. ²⁵ Koma muchoonadi nikuuzani kuti kunali mazenela yambiri mu Izilaeli munthawi ya Elijah, pamene mulengalenga unavaliwa zaka zitatu ndi makakumi asanunu ndi kamozi, ndiponso njala yaikulu inagwela pantaka ija. ²⁶ Koma Elijah sianatumiwe kulialionse, koma chabe ku zerepata wa mu sidoni, kuli ofedwa wamene analikunkhala kuja. ²⁷ Ndiponso kunali akungu ambiri mu Izilaeli ija nthawi ya muneneli Elisha, Koma kulibe anachilisiwapo kucheselako Namani waku sirian." ²⁸ Banthu bonse musinagogi anazozedwa ndi ukali pamene anamvela izi zinthu. ²⁹ Onse anachamuka, ndikumupatikiza kuchoka mumuzinda, ndiponso anamusogolela pamwamba pa phiri kwamene muzinda unamangiwa, kuti bamutaye kuchokela pamwamba paphiri. ³⁰ Koma anapitila pakati kao ndikuenda kumaloena. ³¹ Ndipo anaenda kukapenamu, muzinda wa mu Galilileyo, ndiponso anayamba kubapunzisa paza sabata. ³² Anadabwisiwa pakupunziza kwake, chifukwa anali kunena ndi ulamulilo. ³³ Koma mumasinagogi kunali mwamuna wamene anali namuzimu onyansa, ndiponso analila ndi liu lapamwamba, ³⁴ "Ah! nanga nichani chamene tingachite na iwe, Yesu waku Nazareti? Kodi wabwela kutiononga? Niziba kuti ndiwe _ oyela wa Mulungu." ³⁵ Yesu anazuzula muzimu onyansa, ndikunena, "Osakambe kuti chokamo mwaiye!" Pamene muzimu onyansa anagwesa mwamuna pansi pakati paiwo, anachoka mwa iye, ndiponso sianamuononge munjila iliyonse. ³⁶ Banthu bonse banadabwa, ndiponso anapitiliza kukambapo pali izi kuliwina ndi muzake. Bananena kuti, Kondi ni mau yabwanji aya? Alamulila ndi mizimu zonyansa ndi ulamulilo ndipo ndi mphamvu ndiponso zichoka." ³⁷ Ndiponso utenga pali iye unayamba kuyenda pasogolo pamalo yaliyonse yanazungulila yaja malo. ³⁸ Ndiponso Yesu anaenda choka musinagogi ndiponso anangena munyumba ya Simoni. Koma bapongozi ba Simoni bakazi analikuvutika ndimatenda, ndiponso anabapapatilako. ³⁹ Koma anaimilila pali iye ndiponso anazuzula matenda, ndiponso yanatuluka mwaiye. Pameneapo ananyamuka ndiponso anayamba ndi kuatumikila. ⁴⁰ Pamene zuba anali kungena, banthu onse analeta odwala kuli Yesu anali ndimatenda osiyanasiyana. Anafaka zanja palialionse ndiku achilisa. ⁴¹ Mizimu zonyansa nazo zinachoka mulibambiri, na kulila ndikunena kuti, "Ndiwe mwana wa Mulungu." Yesu anazuzula mizimu zonyansa ndiponso sianazisilile kukamba, chifukwa anaziba kuti ndiwe Kristhu. ⁴² Pamene nthawi yamuzuba inafika, Anayenda mumalo

yobisika. Banthu bambiri banali kumusakila ndiponso anabwela kumamalo kwamene enzelili. banayeselela kumulesa kuti asayende nakubasiya.⁴³ Ndiponso ananena kwaiwo, " Nifunikilanso kulalikila utenga wabwino pazaufumu wa Mulungu kumizinda zinangu, nichifukwa chaichi ninatumiwa." ⁴⁴ Ndipo anapitiliza kulalilila mumasinagogi mumalo yonse ya mu judeya.

Chapter 5

¹ Koma chinachitika kuti, pamene banthu bambiri analikuzingulila Yesu ndiponso kumvelela kumau ya Mulungu, analikuimilila pa nyanje ya Genazareti. ² Anaona maboti yabili yamene analikudonseledwa pamwamba ndikuya chosanakupeleka kumbali yamusinje. Baja bogwila nsomba ninshi bachokamo kudala ndiponso anali kusuka vogwililamo nsomba. ³ Yesu anangena mu boti ina, yamene inali ya Simoni, ndiponso anamufunsa kuchosamo mumanzi pamalo yafupika muliyaja malo. Komanso anankhala pansi ndi kubauza bonse banali muboti. ⁴ Pamene anasiliza kukamba, Ananena kuli Simoni, "Tenga boti ndiponso uipeleka pamanzi yamene yalimumalo mombila maningi pakuti mugwile." ⁵ Simoni anayankha ndikunena kuti, "Mfumu, tasebenza usiku onse, ndiponso sitinagwilepo kalikonse, koma kamba kamau yanu, nizangenesa zogwililamo nsomba pamanzi yombila." ⁷ Pamene bana chita izi, bana unjika nsomba zambiri, ndiponso zogwililamo zao zinali kung'ambika. ⁶ Koma banaenda kulibanzao bamene banali muboti inangu kuti babwele babatandizile. Banabwela ndiponso bana zuzha maboti yonse yabili, chakuti yanayamba nakumbila. ⁸ Simoni Petulo, pamene anaona ichi, anagwela pansi pamapazi ya Yesu, ndikunena, "Chokani paliine, chifukwa ndine munthu ochimwa, Ambuye." ⁹ Chifukwa chinamudabwisa, ndiponso ndi iwobamene analinabo, pakugwila kwansomba zamene banatenga. ¹⁰ Aba banali kuikilako Yakob ndiponso Yoani, mwana mwamuna wa Zebedi, bamene banali kugwilizana nabopamozi ndi Simoni. Ndiponso Yesu ananena kuli Simoni, "Usayope, chikukwa kuchokela manje uzayamba kugwila banthu." ¹¹ Pamene banaleta zongwililamo nsomba kunthaka, banasiya zonse ndikumukonka. ¹² Chinabwela chachitika kuti pamene akali mumuzinda winangu, Munthu wamene anali ndi lepulosi analipo, Pamene anaona Yesu anagwesa manso yake ndi kumupempha, nakunena, "Abuye, ngati mufuna, nitubiseni." ¹³ Ndipo Yesu antambusula kwanja kwake ndi kumugwila, nakunena, "Nifuna, nkhalo otubisiwa." ¹⁴ Anamuuza kuti asauze aliyense, Koma anamuuza, "Kuti enda njila yako, Ndiponso ukazilangize kuopeleka ansembe ndiponso upeleke chansembe pakutubisiwa kwako, kulinganiza mwane mose analamulila, monga umboni kwaiwo." ¹⁵ Koma mbiri paliye anamwazikana patali, Ndiponso magulu yabanthu bambiri benzebanabwela kumvela vamene enze kupunzisa ndiponso anachilisa bambiri bamene benze bodwala. ¹⁶ Koma anali kuchokapo nthawi yambiri nakubasiya noenda mumalo yobisika mukupempela. ¹⁷ Chinabwela chachitika chakuti, muyaja masiku yamene analikupunzisa, Ndiponso kunali afalisi ndi apunzisi amalamulo analichinkhalile kwamenekuja amene anabwela kumalo yambiri yaminzi zosiyana muzigao zija za muGalileyo ndiponso mu Judeya, ndiponso mumunzi wamu Jelusalem. Mphamvu za Mulungu zochilisa zinali paliye. ¹⁸ Koma bamuna bena bana bwela, ananyamula pampasa mwamuna wamene sianali kuyenda, Ndiponso anaona njila yomubwelelamo mukati pakuti amufake kuntangu na Yesu kuti amufakepo zanja. ¹⁹ Sibana pezenjila yomupelekelamo mukati chifukwa kunali chigulu chabanthu, kamba kaichi banaenda pamwamba pa nyumba ndiponso banamuselusila pansi, pa mpasa yake, pakatika banthu, pantangu pamene analili Yesu. ²⁰ Pakuona chikulupilo chao, Yesu ananena, "Mwamuna, machimo yako yakululukidwa." ²¹ Akalembela ndiponso Afalisi banayamba kufunsa izi, ndikunena, "Kodi ni ndani uyu wamene akamba manyozo? Ni ndani angakululukile machimo koma Mulungu eka?" ²² Koma Yesu, pakuziba zamene banali kuganiza, anayankha ndi kunena kwaiwo, "Kodi nichani chamene mufunsila izi mumitima yanu?" ²³ Nanga nichani chopepuka kunena, 'Kuti machimo yako yakululukidwa' loka kunena, 'Kuti ima uyende?' ²⁴ Koma kuti muzibe kuti mwana wa Munthu alina ulamulilo pazikolapansi kukululukila machimo, 'Ninena kwa iwe, 'Nyamuka uime, 'Tenga mpasa yako uyende ndiponso uyende kunyumba kwako." ²⁵ Pamene apo anapita kuntangu kwao na kunyamula mpasa yamene analikugonapo. Ndiponso anabwelelamo kunyumba kwao, ndikutamanda Mulungu. ²⁶ Alionse anadabwa ndiponso banalemekeza Mulungu. Banazozedwa ndi kuyopa, nakunena, "Kuti taona zinthu zamene zopambana lelo." ²⁷ Pochoka kuchitika zinthu izi, Yesu anachoka mumalo yaja ndiponso anaona wamusonko zinalake ni Levi Analinkezi pajapa tenti pamene batengela musonko. Ananena kwaiye, "Nikonke ine." ²⁸ Pomwepo Levi anaima ndiponso anamukonka, ndikusiya zonse pambuyo. ²⁹ Koma Levi anapasa pwando ikulu kuli Yesu munyumba yake. Kunali bamisonko bambiri kujakumalo ndiponso banthu benangu banali kufendela kufupi na tebulo nakuyamba kudya ndi iye. ³⁰ Koma bafalisi ndiponso bakalembela banali kudandaula kubophunzila bake, nakunena, "Kuti kodi nichani chamene udyela ndi kumwa nabamisonko ndiponso ndi ena ochimwa?" ³¹ Yesu anabayankha, "Kuti banthu bamene sibana dwale sibangafune obachilisa, koma chabe bamene bodwala ndiye bangafune. ³² Sininabwele kuitana bathu bolungama kulapila, koma kuitana ochimwa kulapila." ³³ Ananena kwaiye, "Kuti ophunzila ba Yoani bamakonda kupempela ndi kusala kudya kambiri, ndiponso ophunzila abafalisi bachitachimozimozi. Koma afalisi bako bakudya na kumwa." ³⁴ Yesu ananena kwaiwo, "Kodi munthu angapange ukwati wa banthubake bamukwati nakubaleka kutibasale kudya, pamene mukwati akalinabo?" ³⁵ Koma masiku yazabwela pamene mukwati azatengewa kwaiyo, Ndiponso masiku yaja bangasale kudya. ³⁶ Koma Yesu ananena kwaiwo mukanthano. Kulibe anga ng'ambe chinyula

muzigao kuchoka kuchanyowani ndiponso kusebenzesa kutungila kuchovala chakudala. Ngati anachita izi, Afunika ang'ambe chanyowani, Ndiponso chigao chanyula kuchoka kuchanyowani, sichinga fanile ndi chinyula chakudala.³⁷ Ndiponso kulibe angafake vinyu vanyowani mu vinyu vachikumba chakudala. Ngati angachite ivo, Ninshi vinyu vanyowani vinga pwaye chikumba.³⁸ Koma vinyu vasopano vifunika kufaka muchikumba chanyowani.³⁹ Ndiponso kulibe anamwa vinyu vakudala wamene angafune kumwa vanyowani, chifukwa anena, " Kuti vakudala vilibwino."

Chapter 6

¹ Manje chinabwela chachitika pa sabata kuti Yesu analikuyenda mumunda mwamene balima mbeu ndiponso bopunzila bake banali kudoba mitu zambeu, ndikuzinyanyaula mumanja yao ndiponso banalikudwa izi mbeu, ² Koma wina wa afalisi ananena, "Kodi nichifukwa chachani chamene muchitila chinthu chamene sicholamulidwa kuchita pasikula sabata?" ³ Ndiponso pakumuyankha iye, Yesu ananena, "Kodi siunabelenge vamene David anachita pamene enze nanjala, Iye ndiponso nabamene analinabo?" ⁴ Anaenda munyumba ya Mulungu, nakutenga mukate wamene unali munso yake ndi kudyapo mbali yamukate, ndiponso anatengapo mukate wina nakupasa amuna bamene analinao kuti badye, angankhale chinali chabe chovomelezewa kuopeleka ansembe kudya." ⁵ Ndiponso ananena kwaiyo, "Kuti mwana wamuthu ni Mulungu wa sabata." ⁶ Chinachitika pa sabata inangu pamene anaenda musinagogi ndi kuuza banthu bena muja. Munali mwamuna muja wamene anali nanzalamanja lolemala. ⁷ Akalembela ndi afalisi analikumuyangana chabe pafupipafupi nakuona ngati azapolesa wina pasabata, pakuti bapezelepo chifukwa chomuzuzulilapo. ⁸ Koma anaziba zamene banali kuganiza ndiponso ananena kuli mwamuna wamene kwanja yake inali yolemala, "Anati ima, ndiponso uimilile pakati palialionse." Ndiponso mwamuna anaima ndiku imilila pamene paga. ⁹ Yesu ananena kwaiwo, "Nikufunsa iwe, Kodi sicholamulidwa pasabata kuchita zabwino kuchila kuchita voipa, kupulumusa moyo kuchila kuuononga?" ¹⁰ Ndiponso anayanga baja bonse banamuzungulila ndikunena ku mwamuna, "Tambusula kwanja yako." Anachita chomwecho, ndiponso kwanja kwake kunabwezewa. ¹¹ Ndiponso banazozedwa naukali ndiponso ananena kuliwina ndi muzaka chamene bangamuchite Yesu. ¹² Chinabwela chachitika masiku yaja nichakuti anaenda kuluphiri kupempela. Anapitiliza kupempela kwa Mulungu usiku onse. ¹³ Pamene kunali muzuba, anaitana opunzila bake, ndiponso anasankha kumi ndi tuwili bamene analikuitana ati maapostoli. ¹⁴ Mazina yama apostoli banali Simoni (wamene anainika ati Peter) ndiponso abale bake, Andeleo, Yakobu, Yoani, Philipo, Batilomeo, ¹⁵ Mateyo, Tomasi, Yakobu mwana wa Alifas, Simon wamene anali kuitananiwa Ziloti, ¹⁶ Judasi mwana wa Yakobu, Ndiponso Judasi Esikalyoti wamena anali ogulisa. ¹⁷ Koma Yesu anabwela pansi paluphiri ndi iwo nakuimilila pamalo pamene panali polingana ndi ophunzila bake bambiri ndiponso gulu ikulu yabathu baku Judeya ndiponso Jelusalemu ndiponso akuchimana chaku Tyre ndiponso Sidoni. ¹⁸ Banabwela kumvelela kwaiye ndiponso kuchilisiwa kumatenda yao. Banthu bamene anavutisiwa ndi mizimu zonyansa anachilisiwa. ¹⁹ Alionse mugulu analikuyeselela kumugwila chifukwa mphanvu zochilisa zinalikuchoka mwaiye, ndiponso anabachilisa bonse. ²⁰ Ndiponso anayanganila paophunzila bake, ndi kunene, "Ndimwe odala imweamene aliosauka, chifukwa ufumu wa Mulungu ndiye wanu. ²¹ Ndimwe odala bamene mulinanjala, chifukwa muzazozedwa. Ndimwe odala imwe bamene mulila, chifukwa muzaseka. ²² Ndimwe odala ngati banthu banthu bakuzondani ndiponso kukupatulani ndiponso kukutukwanani, chifukwa chamwana wa munthu. ²³ Sekelelani muli ija siku ndiponso ndi chimwemwe, chifukwa muzankhala ndi mphanvu yaikulu kuchoka kumwamba, ndi mibado yao inachita kuaneneli babo munjila imozimozi. ²⁴ Koma vuto ilikuli imwe bamene olemela, chifukwa mwalandila kudala tontozo lanu. ²⁵ Vuto ilikuli imwe bamene aliokutika manje, chifukwa muzamvela njala pasogolo. ilikuli imwe bamene baseka manje, chifukwa muzalila malilo pasogolo ²⁶ Vuto lili kwainu bamene banthu banena zabwino paliimwe, chikukwa iyo ndiye njila mwamene mibado yanu inivutisilamo ananeneli baboza. ²⁷ Koma ninena kwainu bamene bamvela, kondani badani banu ndiponso mubachitile vabwino baja bamene bakuzondani. ²⁸ Dalitsani baja bamene bakutembelelani ndiponso mubapempelele baja bamene bakuvutisani. ²⁹ Kuli iwo bamene bakumenyani kutobo, mupasenso ndi kwinakwache. Ngati munthu wina atenga koti yako, usagwilililenso chovala chako. ³⁰ Pasa aliyense wamene akupempa. Ngati munthu wina atenga chinthu chako, usamufunse kuti akubwezele. ³¹ Monga mwanene ufuna banthu bena kukuchitika, Naiwe uchite chimodzimidzi kulibemve. ³² Ngati ukonda chabe baja bamene bakukonda, Kodi nipindu bwanji yamene ingankale kwaiwe? chifukwa ndi ochimwa akonda kuchita chimodzimidzi. ³³ Ngati uchita vintu vabwino chabe kuli baja bamene bakuchitika vabwino iwe, nanga pindi kuli iwe ni chani? ³⁴ Ngati ukongolesa chabe kuli banthu bamene uganizila kuti ndibemve bazakubwezelanso, Kodi nipindu bwanji iyo kuliwe? Ndi ochimwa amakongolesa kuochimwa, kuti alandile mumuyeselo umodzi. ³⁵ Koma kondani adani banu ndiponso bachitilani vabwino. Kongolesani koma musaganizile kulandila chilichonse ndiponso mphanvu yanu izankhala yaikulu ndiponso muzankhala bana babapamwamba, chifukwa iye mwinewake niwabwino kulibaja banthu bamene sibayamika ndiponso kuli boipa. ³⁶ Nkalani bachifundo, monga mwamene tatewanu ali wachifundo. ³⁷ Musaweluze, ndiponso simuzaweluzidwa, musasule, ndiponso naimwe simuzasuliwa. Kululukila benzanu ndiponso naimwe muzakululukidwa. ³⁸ Pasani, ndiponso naimwe musapasidwa. mumueselo umodzi ndi chisangalalo nakusindila pansi, ndiponso kuzisunkhani pamodzi ndiponso nakutaikila-zizatikila mumanja mwako. Koma mumuyeselo wamene muzasebenzesa, chizabwezedwa kwaiwe. ³⁹ Ndiponso anabauza fanizo, "Kodi nanga munthu osaona angasogolele muzake wamene siaona? ngati

angachiti, Ndiponso bonse bazagwela mumugodi, kodi simwamene?"⁴⁰ Ophunzila simukulu kupambana muphunzisi, koma alionse ngati afikapo pakuphunzisiwa azanhkala monga muphunzisi wake.⁴¹ Ndiponso nichifukwa chani muyanganila pakanthu kang'ono kali mulinso lamubale wako, Koma iwe siunazindikila mutengo ukulu mulinsolako?⁴² Ungakambe bwanji kumubalewako, mubale, 'Lekanichose kanthu kang'ono mulinsolako; ngati iweweka siungaone chimutengo chikulu mulinsolako? Imwe onama! choyamba chosa chija chimutengo chikulu mulinsolako, ndiponso uzaona bwinobwino pakuti uchose kaja kumutengo kang'ono mulinso lamubale wako.⁴³ Koma kulibe chimutengo chabwino chamene chingabeleke zipaso zoola, angankale chimutengo choola chamene chingabeleke zipaso zabwino,⁴⁴ Koma chimutengo chilichonse chizazibika kulinganiza nazipaso zamene chibeleka. Banthu sibama kolola visipo kuchimutengo chaminga zamusanga, angankhale kukolola magrepusi ku mabriya yamusanga.⁴⁵ Munthu wabwino kuchokela muchipao chaubwinowake wamumutima amabeleka za bwino, ndiponso munthu oyipa kuchokela muchipao chakuipa kwamumutima wake amabeleka zoipa. Koma kuchokela mu unyini waza mumutima kamwa kazanena.⁴⁶ Nichifukwa chani chamene muniitanila, 'Ambuye, Ambuye,' ndiponso simumvelela zinthu zamene nikuuzani?⁴⁷ Alionse wamene abwela kwaine ndiponso nakumvelela mau yanga, Nizakuuzani mwamene alili.⁴⁸ Ali monga munthu wamene amanga nyumba, wamene anakumba pansi pantaka ndiponso nakumanga chi manyumba pamwala olimba. pamene kuziliwa kwamanzi kunabwela, kupopota kwamanzi kunachaya nyumba ija, koma siinagwedezake, chifukwa yenze inamangiwa bwino.⁴⁹ Koma munthu wamene amvela mau, ndiponso siyamvelela, alimonga munthu wamene anamanga nyumba pamwamba pantaka kopanda chiyambi. pamene kupopota kwamanzi kunachaya munyumba, pamene apochabe inagwa, ndiponso chibadwile chaija nyumba chinasila."

Chapter 7

¹ Pamemene Yesu anasiliza zonse zamene analikunena mukumvela kwabanthu, anangena mu kapenamu. ² Koma musenchulion anali ndi kapolo wake wamene anakwezewa ngi iye, ndiponso analiodwala pafupi nakufuna kufa. ³ Pamene musechulyoni anamvela paza Yesu, anatuma kwaiye akulu bama jews, nakumufunsa kuti abwele achilise wanchinto wake. ⁴ Pamene banabwela kuli Yesu, Banamufunsa mosilizika, ndikunena, " Nioyenela kuti iwe umuchitile izi, ⁵ chifukwa akonda zikolatu, ndiponso niwamene anatimangila sinagogu yatu." ⁶ Pokapo Yesu anapitiliza munjila yake ndibemve. Koma pamene akalibe kufika patali nanyumba, Uja musenchulyoni anatuma banzake kuli iye, " Ambuye, musazivutise, chifukwa inesindine oyenela kuti mubwele munyumba yanga. ⁷ Kamba kachamene ichi sininazione kuti ndine oyenela kuti mubwele kwaine, Koma kamabani chabemau ndiponso wanchinto wanga azapola. ⁸ chifukwa naine ndine munthu wamene alamulila asilikale. Nimane kuli uyu, 'kuti enda', ndiponso ayenda, ndiponso amanena kuli wina, ' bwela, 'ndiponso abwela, ndiponso kuli wanchito wanga, ' chita ichi, 'ndiponso amachita," ⁹ Pamene Yesu anamvela izi, Analiodabwisiwa ndi iye, ndiponso pakubwelela ku gulu lamene linali kumukonka, " Ndikunena kuti, nikalibekupezapo chikululupilo monga ichi mu Izilaeli." ¹⁰ Ndiponso banebenze naye banatumiwa kubwelela kunyumba, ndiponso banapeza kuti wanchito alibwino. ¹¹ Kuchekela pamene apo Yesu anaenda kumuzinda wina oitanidwa Nani, Ndiopunzilabake ndiponso nagulu ikulu inaenda ndi iye. ¹² Pamene anafika pafupi ndikomo yamuzinda, Koma, mwamuna enzeokufa ananyamulidwa kuenda kunja, mwana mwamunaeka wamene bamaibake banali naye (wamene anali ofedwwa), ndiponso gulu ikulu kuchoka mumuzinda banali ndi iye. ¹³ Pamemene ambuye anamuona, Analiotengedwa ndichifundo paliemve ndiponso ananena kwaiye, " kosalila." ¹⁴ Ndiponso anapita kugwila mapulanga mwamene bananyamulila tupi, ndiponso bamene bana nyamula banaimilila. Ananena kwaiye, mwamuna wachichepele, ninena kwaiwe, nyamuka." ¹⁵ Mwamuna wakufa anankala nakuyamba kukamba, ndiponso Yesu anamupasila kuli bamai bake. ¹⁶ Ndiponso bonse banagwilidwa ndi mantha, ndiponso banapitiliza kutamanda Mulungu, nakunena, " Kuti muneneli mukulu anyamulidwa paliise" ndiponso " Mulungu ayanganila bana bake."

¹⁷ Uyu utenga wabwino pali Yesu unasalangana konse mu Judeya ndiponso kulionse uzungulila zigao. ¹⁸ Aphunzila ba Yoani anamuza palizonse izi. ¹⁹ Ndiponso Yoani anaitana ophunzila bake babili ndikubatuma kwa ambuye ndikunena, " Kodi ndimwe amene mufunika kubwela, olo tiyangani kuli winangu?" ²⁰ Pamene bana bwela pafupi ndi Yesu, Azimuna ananena, " Kuti Yoani mubadizi atituma kwaiwe ndikunena, ' Kuti kodi ndiwe wamene azabwela, olo tiyanganile winangu?" ²¹ Paliija nthawi anachilisa banthu bambiri banalnda ndiponso analiomangidwa ndiponso kumizimu zonyansa, ndiponso kupasa menso kuosaona. ²² Yesu anayankha ndikunena kwaiwo, " pamene muzaenda munjila yanu, mukamu uze Yoani zamene mwaona ndiku mvela. bakungu bapenya, olemala alikuenda, bodwala kate batubisiwa, ovala matu bamvela, bakufa baukisiwa nakubwelela kumoyo, ndi aja opelebeli auziwa utenga wabwino. ²³ Munthu wamene siasiya kukulupilila mwaine chifukwa chazinthu zamene nilikuchita niodalisika." ²⁴ Kuchoka pamene batumiki ba Yoani bana enda, Yesu anayamba kunena pali Yoani, " ²⁵ Nichani chamemene mwenzemwaendela panja muchipululu kuona? matete ananyan'ganisiwa ndi mpepo? Nanga wenze waenda panja kuona chani? Mwamuna ovala vovala vabwino? Onani, baja bamene bavala vovala vodula nabaja bamene bankala mankalidwe yapa mwamba bankala mumanyumba ya ufumu. ²⁶ Koma mwenze maenda kuona chani? Muneneli? Eeh, ikuuzani imwe, naku chilapo pali muneneli. ²⁷ Uyu ndiye wamene vinalembewa kuti, 'Ona, Nituma mutola nkani kukusogolela, wamene azakukonzela njila.' ²⁸ Niku uza iwe, pali bantu bamene banabadwa kuli bakazi kulibe mukulu ochila Yohane. Koma uja wamene nimung'ono mu ufumu wa Mulungu nimukulu kumuchila eve. ²⁹ (Pamene bantu bonse banamwela ichi, pamozi na bamisonko, banakamba kuti Mulungu niolungama, chifukwa banabatiziwa na ubatizo wa Yohane. ³⁰ Koma ba Falisi na bozibisisa malamulo banakana lingo ya Mulungu pa myoyo zabo, chifukwa sibana batiziwe na Yohane.) ³¹ "Nanga nikuli chani, manje, chamene ninga linganzane uyu mubadwe? ³² Uli monga chani kansu? Uli monga bana bamene basobela kumalo kogulisilako, bamene bakankala pansu baitanana wina na muzake kukamba kuti, 'Tinakulinzila mutolilo iwe, koma siuna vine. Tinaimba nyimbo ya malilo, koma iwe suna lile.' ³³ Chifukwa Yohane mubatizi anabwela sanali kudya buledi kapena kumwa vinyu, koma imwe mukamba kuti, 'Ali na chibanda.' ³⁴ Mwana wa Muntu anabwela mokudya na kumwa, imwe mukamba kuti, muzake waba misonko na bama chimo!" ³⁵ Koma nzelu zima weluzika zolungama na bana bake bonse." ³⁶ Manje umozi wa a Falisi anaitana Yesu kuti akadye naye. Pamene Yesu anangena mu nyumba ya mu Falisi uja, anankala podyela kuti adye. ³⁷ Onani, kunali mukazi wina mu muzinda wamene anali wama chimo. Pamene anaziba kuti ana nkala podyela munyumba ya mu Falisi, anabwelesa mpika munali mafutga yonunkila. ³⁸ Pamene ana imilila kumbuyo kwake, anali kulila, anayamba kunanisa mendo yake na misozi, nakuya puputa

na sisi zake naku mpyompyona mendo nakuya zoleka na mafuta yonunkila.³⁹ Pamene uja mu Falisi wamene anaitanila Yesu anaona ichi, anaganiza mumutima mwake kuti, "Ngati uyu mwamuna ni muneneli, aseme amuziba uyu muntu na kuti ni muntu wamu nkaliidwe bwanji wamene amugwila, chifukwa niwama chimo."⁴⁰ Yesu anamuyanka kuti, "Simoni, nili na chintu chamene nifuna kuku uza iwe." Anamuyanka kuti, "Kambani, Apunzisi!"⁴¹ Yesu anakamba kuti, "Muntu umozi okongole ndalama anali na babili ba nkongole. Umozi anali na nkongole zokwanila 500 dinari, wina 30."⁴² Pamene banakangiwa kubweza nkongole, anabakululukila bonse. Mwa ichi, pali aba niuti wamene azamukonda maningi?"⁴³ Simoni anamuyanka kuti, "Niwona monga ni uja wamene anamukululukila zambili." Yesu anamu uza kuti, "Waganizila bwino."⁴⁴ Yesu anapindamuka kulangana mukazi uja naku uza Simoni kuti, "Wamu ona mukazi uyu. Ine nangea munyumba mwako. Siunani pase manzi yosambila kumendo, koma eve ananisa mendo yanga na misozi zake naku ya puputa na sisi zake."⁴⁵ Iwe siunani mpyompyone, koma kuchokela pamene ine nabwelela eve sanaleke ku mpyompyona mendo yanga.⁴⁶⁴⁷ Iwe siuna zoleke mutu wanga mafuta, koma eve azoleka mendo yanga na mafuta yonunkila. Chifukwa chake niku uza iwe kuti, machimo yake, yamene yanali yambili, yakululukiliwa-chifukwa eve akonda maningi. Koma wamene akululukiliwa tung'ono, amakonda pang'ono."⁴⁸ Anamu uza mukazi uja kuti, "Machimo yako yakululukiliwa."⁴⁹ Baja bamene banali nkale podyela pamozi na eve bana yamba kukamba pakati pabo kuti, "Kansi nindani uyu wamene akululukila namachimo?"⁵⁰ Yesu anauza mukazi uja kuti, "Chikululupililo chako chakupulumusa. Enda mwamu tendele."

Chapter 8

¹ Chinabwela chachitika kuchokela apa kuti Yesu anayamba ulendo mu mizinda yosiya-siyana na minzi, kulalikila na ku ulusa utenga wabwino wa wamulungu. Bopunzila kumi na babili banali na eve, ² na bazikazi bena bamene banachilisiwa ku mizimu zonyansa na kumatenda: Maliya wamene analikuitanidwa Magadalena, wamene anachosewamo mizimuzonyansa zinali tusanu nditubili; ³ Yoana mukazi wachuza, Mukulu paoyanganila wa Herode; Suzeni, ndiponso nabengu bambiri, bamene, mukuchokela muzimene banalinazo, anasamalila zofunikila zao. ⁴ Pamene gulu ikulu yabanthu yenzeli kukumana, na banthu benze kubwela kuchokela mumizinda, anabauza fanizo: ⁵ "Mulimi anaenda kushanga mbeu. Pamene enzeli kushanga, zinangu zinagwela mumbali mwa njila na kudyakiwa, na nyoni zamumwamba zina zidya. ⁶ Zinangu zinagwela pa mwala, na pamene zina kula chabe, zinayuma, chifukwa zinalibe manzi. ⁷ Zinangu zinagwela pa minga, minga zinakula pamozi nambeu na kulasa mbeu zija. ⁸ Koma zinangu zinagwela panthaka ya bwino naku mela naku bala vipaso vambili." Pamene Yesu anasiliza kukamba ivi vinthu, anabaitana kuti, "Aliense wamene alina matu yakumvela, lekani amvele." ⁹ Bophunzila beke banamufunsa chamene fanizo iyi itanthauza. ¹⁰ Anaba yankha, "Kuziba kwa visinsi vaufumu wa Mulungu kwa pasiwa kuli imwe, koma kuli benangu nikamba muma fanizo, kuti 'kuona sibangaone, na kumvela sibanga mvesese.' ¹¹ Manje iyi ndiye tanthauzo ya fanizo. Mbeu ni mau ya Mulungu. ¹² Zamene zili mumbali mwanjila nibaja bamene bamvela, koma mudyelekazi abwela nakutenga mau mumitima yao kuti bsakhulupilile naku pulumusiwa. ¹³ Zamene zili pa mwala nibaja bamene, bakamvela mau, bayalandila nachimwemwe. Koma balibe muzyu; bakhulupilila kanthawi kangono, dipo munthawi yama yeso wamagwa. ¹⁴ Mbeu zamene zinagwela pa minga nibaja banthu wamne bamvela mau, koma pamene baenda, balasiwa navo desankhaba na chuma na vomvesa bwino thupi vaumoyo una, ndipo vipaso vao sivikiphya. ¹⁵ Koma mbeu zamene zina gwela pa nthaka yabwino, abo nibaja bamene, bamvela mau muchilungamo na mutima wabwino, kuya gwililila na kubala vipaso mukuyembekeza nakupilila. ¹⁶ kulibe wamene amayasha nyali nakuivinikila na mbiya kapena kufaka pansi pa bedi. koma, amaifaka pachokapo nyali kuti aliyense wamene angena aone kuunika. ¹⁷ pakuti kulibe chobisika chamene sichizakazibika, kapena chisinsi chilichonse chamene sichizakazibika naku bwela poonekela. ¹⁸ Manje nvesesani, kuliwamene alinavo, vinangu vizapasiwa kuli eve, koma wamene alibe, navonse vame aganiza kuti alinavo vizapokewa kuchoka kuli eve. ¹⁹ Kuchoka apo amai baka naba bale bake bana bwela kuli iye, koma sibana kwanise ku fika pafupi naye chifukwa chakupaka kwa bantu. ²⁰ Anauziwa, "Amayi bako naba bale bako bali imilile panje, kufuna kukuona." ²¹ Koma Yesu anayanka naku kamba kuli beve kuti, "Amayi banga naba bale banga ni abo bamene banvela mau ya Mulungu naku yachita." ²² siku imozi ana kwela mu bwato nabo punzila bake, ndipo anabauza kuti, "tiyeni kumbali inangu kwa nyanja." Banayambako. ²³ Koma pamene banali kuyenda mubwato iye anagona. kunabwela chimpepo chikulu pa nyanja, namu bwato mwao munayamba kuzula manzi, ndipo banali mu chiyopezo. ²⁴ Ndipo bophunzila ba Yesu bana bwela kuli eve na kumu usha, kukamba kuti, "Ambuye! Ambuye! Tili pafupi nakufa!" Anauka na kukalipila chimpepo na manzi yenze kunyamuka, vinaleka, ndipo kunali mutendele. ²⁵ Ndipo anakamba kulibeve, "Chukhulupililo chanu chili kuti?" Koma bana yopa naku dabwa, naku funsana wina namunzake, "Kansi uyu nindani, wamene alamulila mphepo na manzi, ndipo vimumvelela?" ²⁶ Bana yenda pamanzi kumalo ya Gerasenesi, yamen yali ku mbali inangu ya Galilea. ²⁷ Pemena Yesu anaseluka mu bwato, anakumana na mwamuna winangu wamene anili na vibanda. Kwa nthawi itali sanavalepo vovala, ndipo senzo nkhalamunymba koma pakati ka manda ²⁸ Pamene anona Yesu, analila nagwa pansi pamaso pake na kukamba mokuwa, "Muzachita chani naine, Yesu, Mwana wa Mulungu Mukulu? Nikupephani, musani nzunze." ²⁹ Chifukwa Yesu analamulila muzimu oipa kuti uchoke muli uja munthu. Ndaba nthawi zambili wanzo mugwila, nagu enzeli omangiwa nakulondewa, enzodula vomumangila ndipo vibanda venzo mulengasa kuyenda musanga. ³⁰ Ndipo Yesu anamufunsa, "Ndiwe ndani?" Anakamba, "Legoni," chifukwa vibanda vambili vinamugena. ³¹ Venze kungu mupapatila kuti asavitume ku gahena. ³² Penzeli nkhumba zambili zenzo kudya kumbali kwa chulu. Vibanda vinamu pempha kuti avivomeleze kuti vingene munkhumba, ndipo anavi vomeleza. ³³ Ndipo vibanda vonachoka muli uja munthu nakungena munkhumba, na gulu yankhumba zija tamanga nakuzi ponyela munyanja nakumbila. ³⁴ Pamene oyanganila nkhumba banaona vame vana chitika, bana thamanga naku uza bamu mzunda na kumbali kwa ziko iyo. ³⁵ Ndipo banthu bana yenda kuti baone vame vachitika, naku bwela kuli Yesa nakupeza munthu wamene vibanda vachokamo. Enze nkhalamunymba pama pazi ya Yesu, wovala na nzelu zake; ndipo mbanamvela mantha. ³⁶ Ndipo bame banaona vinacitika banaba uza mwemene uja munthu enzeli ogwiliwa na vibanda anachilisiwa. ³⁷ Banthu bonse baku dela ya Gerasenesi banamu pempha Yesu kuti achoke kuli beve, chifukwa bana tengeka namantha kyakulu. Mwaicho anagena mu bwato kuti ba bwelele. ³⁸ Munthu wamene vibanda vina choka anamu papatila kuti aende nae, kom Yesu

namubweza, kukamab kuti, ³⁹ "Bwelela kunyumba kwako nakupasa umboni okwanila pali vemen mulungu akuchitila." Uja munthu anayenda, kulalikila mumzinda onse vamene pa vamene Yesu ana muchitila. ⁴⁰ Manje pamene Yesu ana bwelela, gulu ina mulandila, chufukwa benzeli kumu yembekeza. ⁴¹ Onani, munthu zina yake Jailosi, Wamene enzeli umozi waba sogoleli ba sinagoge, anabwela nakugwa pamapzi ya Yesu, nakumu papatila kuti abwele kunyumba kwake ⁴² chifukwa mwana wake mukazi eka, musikana wazaka 12, anali kufa. Pemene yesu munjila, gulu yabanthu inakululako kumu zungulila ^{43 44} Manje penzeli muzimai wmene anzo choka magari zaka 12 ndipo anaziliza ndalama zake zonse, koma sana polesewe na alionse. Anabwela kumbuyo kwa Yesu nakugwila mumbali mwa chovala chake, ndipo pamene apo kuchoka makazi kwake kunaleka. ⁴⁵ Yesu anafunsa kuti, "Nindani wamene ani gwila?" Pamene bonse bana kana, Petulo anamu yankha, "Ambuye, gulu yabanthu yaku zungulilani ndipo bakungo fendela pafupi naimwe." ⁴⁶ Koma Yasu anakamba kuti, "Kuli wamene anigwila, chifukwa niziba kuti mphamvu zachoka muli ine." ⁴⁷ Pamene muzimai anaona kuti sanga thabe, anabwela onjenjemela nakugwa pansu pamenso pake. Pamenso pa banthu nonse anakamba chamen anamugwilila n mwamene anapolela pamene apo. ⁴⁸ Ndipo Yesu anamu uza, "Mwana mukazi, chikhulu pililo chako chakupolesa. Enda mumtendele." ⁴⁹ Pamene akali kukamba, winangu anabwela kuchokela kunyumba ya musogoleli wa sinagoge, "Mwana wako mukazi amwalila. Osavutisa aphunzisi." ⁵⁰ Koma pamene Yesu anamvela ichi, anayankha Jailosi, "Usa yope; khulupilila chabe, ndipo azachilisiwa." ⁵¹ Pamene anafika panyumba, sana vomeleze aliense kungena naeve, kuchoselako Petulo na Yohane na Yakobo, na batate bake ba mwana na bamaibake. ⁵² Manje bonse benzolila mwana, koma anakamba kuti, "Musalile; sanafe agona chabe." ⁵³ Koma banamuseka, kuziba kuti anamwalila. ⁵⁴ Koma anamunyamula nakwanja naku itana, kukamba kuti, "Mwana, imilila!" ⁵⁵ Muzimu wake unabwelela, anaima nakuima pamene apo. Anabauza kuti bamupase chakudya adye. ⁵⁶ Makolo yake banadabwa, koma anabauza kuti basauze muntu ali onse chamene chinachitika.

Chapter 9

¹ Anaitana bopunzila bake bali 12 naku bapasa mpamvu za naulamulilo kuchosa zonse babanda naku polesa matenda yaliyense. ² Anabatuma iwo kulalikila za mfumu wa Mulungu ndi kupolesa odwala. ³ ⁴ Anati kwa iwo, "osatenga chintu chonse paulendo wanu kulibe ndondo kulibe ndaalama ndi nyumba iliyonse yamene muzangena nkalani mwamene mpaka muyende. ⁵ Kulikonse kwamene sibazakulandilani, pamene musiya mizinda nakupukuta doti kumapazi yanu kuchitila uboni kwa iwo." ⁶ Ndipo anayenda ndi kupita ku minzi, kulalikila utenga wabwino ndi kupolesa bonse. ⁷ Ndipo Herodi amanvera zonse zamene zinacjika, ndipo ana dabwa, chifukwa bena bakamba kuti Joni auka kwa akufa, ⁸ ndipo benanso banakamba kuti, Eliya anaonekela, ndi bana nungu bakamba umozi wa aneneli wamene aliko kudala wauka. ⁹ Helodi anakamba, "ninamujuba mutu Joni nanga uyu nindani wamene ninvela achita ivi?" ndipo anafuna kukamuona iye. ¹⁰ Pamene bopunzila banabwelela banamuza enve vonse vamene banachita ndipo anabtenga nakuyenda nabo, nakuyenda mobisama kuziko la betisaida. ¹¹ Koma pamene gulu inamvela vamene ndi kumukoka iye. analandila nakumba nabo zamfumu wa Mulungu nakupolea anafumu kupola. ¹² Koma pamene siku inakuyenda kusuka ndipo anabwela kwa iye na naku kamba, "tumani gulu ichoke kuyenda minzi yozunguluka ndi kumba kwa ziko kuti bapeze kogona na chakudya, chifukwa kunp ndimalo yapayenka. ¹³ Koma anakamba kwa iyo, "uzabapasa zamene bangadya?" bamakamba "tilibe mukate yambili koma chabe 5 na nsomba zibili icepena tiyende kugula vakudya vabantu bonse." ¹⁴ (Bantu bali 5000) bamuna anakamba, "bauzeni bankala pansi gulu iliyonse inkale muma gulu ya 50." ¹⁵ Anachita ichi, anauza kuntala pansi. ¹⁶ Anatenga mukate ili 5 na nsomba zibili anayangana kumwamba, na dalisa na nyama tung'ono napasa iyo bopunzila bake pamozi na gulu. ¹⁷ Onse anadya anakuta na vosala banatenga babasikiti ali 12 zina salako. ¹⁸ Inafika ntawi pamene Yesu anali kumpepela yake, bomunzila bake banali nayenve anabafuna benve, kuti bushe gulu iyi ikamba kuti ndine ndani?" ¹⁹ Gulu inayanka, "Yohani mubatizi. Koma bena banakamba kuti Eliya niumozi wa a neneli bakudala auka. ²⁰ Pamene apo anakamba nabo, "koma imwe mukamba kuti ndine ndani, "Petulo anayanka, "ndimwe Kristu wa Mulungu." ²¹ Koma anachenjeza nakulangiza kuti osauza wina, ²² pakuti mwana mwa muntu afunika kuvutika kukaniwa na bakulu bakulu bansembe na alembi ndi afalisi ndi siku lachitatu azauka. ²³ Ndipo anakamba kwa iyo bonse, "angati alionse afuna kubwela kwaine, afunika kzikana iye yeka nakutenga mutanda wanga nakuninkoka ine. alionse azasunga moyo wake azautaya, ²⁴ koma wamene azataya moyo wake chifukwa chaine azapulumu moyo wake. ²⁵ Nichabwino nichani kutenga zuko lose kapena kutaya moyo wake olo kapena kuononga moyo wake. ²⁶ Uyo aliyense akandinvela manyazi mau anga naiwe wana wamuntu azakakunvela nsoni pamene abwela mu ulemelelo wake, ulemelelo Wabatate bake na ngelo woyela. ²⁷ Koma nikamba kwa iwe zo-ona, kulibena baimilila apa sbazaona ifa, bakalibe kuona umfumu wa Mulungu." ²⁸ Namanje pamene panapita masiku ali 8 Yesu anakamba mau aya, ananyamula Petulo na Joni na Jemusi napita ku pil kukapempela. ²⁹ Pamene anali ku pempela, paso pake pana chinja, nanyula yake inankala yoyela. ³⁰ Onani, bantu babili anali kukamba naye Mose na Eliya, ³¹ anaonekela mu ulemelelo, nakamba nkani yoyambapo iyo yamene yosilizla ku Yelusalemu. ³² Manje Petulo naonse alinali naye anagona tulo to lema pamene banauka bana bonaona ulemelelo bantu babili baimilika pafupi naiye. ³³ Pamene kuchoka kuli Yesu, Petulo anakamba kwa iye "bwana, nichabwino kwise kunkala pano tiyeni timange manyumba yatatu, yinangu yanu, inangu ya Mose, na inangu ya Eliya." (Sanaziba zamene anali kukamba.) ³⁴ Pamene anali kukamba ivi, makumbi yanababuimba naku bachingiliza, na kuyopa pamene bangena mumakumbi. ³⁵ Mau anachoka mumakumbi juti Uyu ndiye mwana wanga wamene bosankawa munveleni iye." ³⁶ Pamene mau yanakamba, Yesu anazipeza yeka onankala zii na sibanauze banaona. ³⁷ Pasiku yokonkapo, anabwela pansi kuchokela ku lupili, chigulu nachigulu chinabwela kukumana naye. ³⁸ Onani, mwamuna mukati mwa gulu amalila kuti mpunzisi, nikaphani kuti muone mwana wanga, ndiye mwanga eka. ³⁹ Yanganani, muzimu utenfa ulamula pali iye posachedwa anapunda, chinalengesa tupi, yake inanyanyaya na pwobu inachoka kukamwa. chinavuta kusiya iye anankala na vilonga vambili. ⁴⁰ Mpepa lophuzila bako bachipatize kuchota koma sibanakwanisa." ⁴¹ Yesubomayanka kuti, "Imwe usakulupilila mubdwo machimo onyonzeka, nankalani naimwe kwa ntawi bwanji? Leta mwana wako apa," ⁴² Pamene munyamata alikubwela, chibanda china mutaya pansi naku mudabwisa monte mela koma anazuzula muzimu wosayela nakumupolesa munyamata nakubapasa batate bake. ⁴³ Pamene apo bonse banadabwa zakulu zamene Mulungu anachita, pamene akali kudabwa navonse anali kuchita anakamba kwa bopunzila, ⁴⁴ "Siyana mau aya yankale mumakutu yanu. mwana wa muntu azapelekewa mumanja ya bantu. ⁴⁵ Koma sibananvele chamene anatantauza china chobisika kwaiwo, sibanazibe itanduzo yake. ndi kuopa kumufunsa chamene anakamba. ⁴⁶ Mwayio banayamba kushushana kuti nindani mukulu. ⁴⁷ Koma Yesu, mukuziba maganizo yabo na mumitima, anatenga kamwana nakafaka pambal pake. Nakamba ⁴⁸ kwa benve, alionse azalandila mwana uyu muzina langa alandila ine;

nawamene alandila ine; alandila wamene anaituma, pakuti mungóno waimwe bonse ndiye mukulu." ⁴⁹ Joni anayanka, "mupunzisi, taona muntu wina achosa madimo mu zia yanu tinamulesa chifukwa sayenda pamozi naife." ⁵⁰ "Usamulesa iye, "Yesu anakamba chifukw samenyana ninshi ali kuli imwe." ⁵¹ Pamene masiku yamafika kuti iye, kutengewa mumbwa. maso yake kuyangana ku Yelusalemu. ⁵² Atuma otumika pasogolo pake paiye ayenda nakungena ku Samatia mizi kukonzeka zonse. ⁵³ Koma bantu kuja sibana mulandile iye chifukwa adaka yabo ku yenda ku Yelusalemu. ⁵⁴ Pamene opunzila Jamesi, Joni anaona ivi anakamba kuti "Ambuye, mufuna kuti tilamulela mulilo kuchoka ku mwamba na kuononga iyo?" ⁵⁵ Koma abwela naku zuzula iyo, ⁵⁶ nakuyenda kumizi yina. ⁵⁷ Pamene banali kuyenda munjila, wina anakamba, kwa iye "nakunkoka kolise muzayenda." ⁵⁸ Yesu anakamba, "Khadwe zili namigodi, na nyoni mu mwamba zili na nchisa, koma mwana wa muntu alibe kogona muntu wake. ⁵⁹ Anakamba winamuza, "Nikonke ine." Koma anakamba Ambuye lekai ine nikaike batate banaga." ⁶⁰ Koma akamba "siyani bakufa bazi ike beka beka, Koma kwa ine nayenda ukalakila patali na patli mfumu wa Mulungu. ⁶¹ Wina mwaiyo anakamba, "nizanku btani, "nizakukonkani, Ambuye koma siyani nikabaila kuli balikunyumba." ⁶² Yesu anayanka kwa iye, "kulibe angatenge kwanja kuika pali choliliila nankuona kumbuyo ninshi akwanisa mfumu wa Mulungu,

Chapter 10

¹ Manje kuchokela apa, Ambuye banasanka benangu bali 70, naku batuma babili balili kubasogolela mu muzinda uli onse na kumalo kwamene beve banali kufuna kuyenda. ² Banabauza kuti, "Vokolola nivambili, koma bokolola nibang'ono. Chifukwa chake pempani ba Mbuye ba vokolola kuti batumize banthito mumunda wabo. ³ Endani njila yanu. Onani, Nakutumani monga nkosa pakati pa mimbulu. ⁴ Osanyamula kasaka kandalama, kapena chola cha uja ali paulendo, kapena nsapato, musapase moni muntu ali onse munjila. ⁵ Nyumba ili yonse yamene mungenampo, poyamba kambani kuti, 'Lekani mutendele unkale panyumba ino!' ⁶ Ngati alipo muntu wamutendele, mutendele wanu uzankala pali eve, koma ngati palibe, uzabwelela kuli imwe. ⁷ Nkalami munyumba yamene ija, kazidyani nakumwa vamene bakupasani, chifukwa wantchito aenela kufola. Osayenda yenda kuchoka mumanyumba. ⁸ Muzinda uli onse wamene mwafikamo, ndipo bakulandilani, dyani vilivonse vamene bakupasani ⁹ nakupolesa bantu bodwala bamene balimo. Bauzeni beve kuti, 'Ufumu wa Mulungu wabwela pafupi naimwe.' ¹⁰ Pamene mungema mumuzinda koma bantu sibakulandilani, endani mumanjila yake nakukamba kuti, ¹¹ 'Na doti yamuzinda yanu yamene yatinkala kumendo ti ichosa kushusha imwe! Koma imwe zibani ichi: Ufumu wa Mulungu wabwela pafupi naimwe.' ¹² Niku uzani kuti pa siku yoweluza chiza wamilako Sodoma kuchila uja muzinda. ¹³ Soka kuli iwe, Kolazini! Soka kuli iwe, Betisaida! Chifukwa asembe ntchito zamene zichitika mukati mwako sembe zinachitiwa mu Tayala na Sidoni, asembe bana tembenulka kudala, nakuvala vovala vama saka na milota. ¹⁴ Koma chizawamilapo Tayala na Sidoni pa siku yoweluza kuchila iwe. ¹⁵ Iwe, Kapenaumu, kansi uona monga uzakwezewa kufika kumwamba? Iyayi, uzabwezewa pansi ku Hadesi. ¹⁶ Wamene amvela imwe amvelela ine, wamene akana imwe akana ine, nauja wamene akana ine akana wamene ananituma ine." ¹⁷ Baja 70 banabwelela nachimwemwe, kukamba kuti, "Ambuye, na vibanda vinazimvelela ise muzina yanu." ¹⁸ Yesu anabauza kuti, "Ninali kuona Satana akugwa kumwamba monga kaleza. ¹⁹ Onani, Nakupasani ulamulilo odyaka njoka pamozi na zinkanila, na pa mpavu zonse za mudani, kulibe chilichonse chamene chizaku onongani imwe. ²⁰ Koma imwe musakondwele chifukwa cha ichi, kuti mizimu zikumvelelani imwe, koma sangalalani kuti mazina yanu yanalembewa ku mwamba. ²¹ Pantawi yamene ija anakondwela kwambili mumu Zimu Oyela, nakukamba kuti, "Nikutamandani imwe, Atate, Mbuye wakumwamba na pansi, chifukwa munabisa ivi vintu ku bantu banzeli na bomvesesa naku vilangisa kuli baja bosapunzila, monga bana bang'ono. Inde, Atate, chifukwa ichi chinali chomvesa bwino mumenso yanu. ²² "Vintu vonse vinapelekewa kuli ine kuchokela kuli ba Tate, ndipo kulibe ali onse wamene aziba Mwana koma ba Tate, ndipo kulibe wamene aziba kuti ba Tate nibati koma Mwana nabaja bamene Mwana anasanka kubazibisa." ²³ Anapindamukila ku bopunzila bake naku bauza mobisila kuti, "Bodalisika nibaja bamene baona vintu vamene muona imwe. ²⁴ Niku uzani kuti, baneneli bambili na mamfumu yambili banafunisisa vintu vamene muona, koma sibanavione, nakumvela vintu vamene mumvela, koma sibanavimvele." ²⁵ Onani, kaswili wamalamulo anaimilila kuti amuyese, kukamba kuti, "Mupunzisi, nichani chamene niyenela kuchita kuti ninkale namoyo wamuyayaya?" ²⁶ Yesu anamu uza kuti, "Nanga nichani chamene chinalembewa muma lamulo? Umavibelenga banji?" ²⁷ Anayanka kukamba kuti, "Ukonde Mbuye Mulungu wako namutima wako wonse, namoyo wako wonse, nampavu zako zonse, na nzeli zako zonse, na muzako monga mwamene uzikondela weka." ²⁸ Yesu anamuyanka kuti, "Wayanka bwino. Chita ichi, ndipo uzankala na moyo." ²⁹ Koma eve, kufuna kuzilungamisa pa eka, anamuyanka Yesu kuti, "Kansi niuti muzanga?" ³⁰ Yesu anayanka kuti, "Muntu wina anali kuyenda kuchoka mu Yelusalemu kuyenda ku Yeliko. Anakumana na vigabenga, vinamupoka katundu wake, nakumumenya, naku musiya kuti afe. ³¹ Pa ntawi wansembe wina anali kupita kunjila ija, ndipo pamene anamuona, anapitila kumbali yina. ³² Chimozi mu Levi, pamene anafika pamalo aya naku muona, anapita kumbali yina. ³³ Koma mu Samalitani winangu, pamene anali pa ulendo wake, anafika pamene analili. Pamene anamuona, anagwiliwa na chifundo. ³⁴ Anamukonka nakumukonza vilonda, kutilapo mafuta na vinyu vosasa. Anamunyamula pa choweta chake, nakumuleta ku malo ya balendo, nakumusamalila. ³⁵ Siku yokonkapo anachosa ndalama za dinali zibili, nakulipila kuli mwine, nakumu uza kuti, 'Musamalile uyu, na vonse vamene uza sebenzesa kuikilapo, nikabwela ine, nizakubwezela.' ³⁶ Nanga pali aba batatu niuti wamene muganizila kuti ndiye ndiye muzake wa uyu anakumana na vigabenga?" ³⁷ Anayanka kuti, "Ni uja wamene anamumvelela chifundo." Yesu anamuyanka kuti, "Enda naiwe ukachite chimozi mu." ³⁸ Manje pamene banali kuyenda, anangena mu munzi uyo, mwamene mukazi umozi zina yake Malita anamulandila munyumba yake. ³⁹ Anali na mubale wake zina yake Maliya, wamene anankala pansi pa mendo ya Ambuye naku mvelela mau yake. ⁴⁰ Koma Malita anali otengewa na kukonza vakudya vomupasa. Anabwela kuli Yesu naku kamba kuti, "Ambuye, nanga kansi simuniganizilako kuti mulongo wanga anisiya neka kukutumikilani? Mu uzeni ani tandizile." ⁴¹ Koma Ambuye banamuyanka kuti, "Malita, Malita, ndiwe wovutika

mutima na vintu vambili,⁴² koma chintu chimozi chabe ndiye chofunikila. Maliya asanka chamene chabwino, chamene sichizapokewa kuli eve."

Chapter 11

¹ Chinachitika siku imozi kuti Yesu anali kupempela mumalo yamozi. Pamene anasiliza, umozi wa opunzila wake anamu uza kuti, "Ambuye, tipunziseni ise kupempela munga mwamene Yohane anapunzisa bopunzila bake." ² Yesu anabayanka kuti, "Pamene imwe mupempela mukazikamba kuti, 'Atate, lekani zina yanu ilemekezewe kuti niyo yela. Lekani ufumu wanu ubwele.' ³ Mutipase ise chakudya chatu chalelo. ⁴ Tikululukileni machimo yatu, munga mwamene ise timakululukila bonse bamene bamatilakwila ise. Musatipeleke ise mumayeso.'" ⁵ Yesu anabauza kuti, "Nanga niuti pali imwe wamene azankala namuzake, wamene azamuyendela pakati pa usiku, naku mu uza kuti, 'munzanga, nibwelekeko mukate utatu, ⁶ chifukwa kwabwela muzanga achoka pa ulendo, nilibe na chilichonse chamene ningamupase chakudya'? ⁷ Pamene apa uja wamene ali mukati anamuyanka kuti, 'Usanivute ine. Chiseko chavaliwa kudala, na bana banga, pamozi naine, bagona kudala. Siningakwanise ku ima kuti nikupase mukate.' ⁸ Niku uzani kuti, ngakale kuti saza ima kuti amupase mukate chifukwa chakuti ndiwe muzake, koma chifukwa chakuti walimbikila kopanda nsoni, azaima nakukupasa mukate munga mwamene wafunila iwe. ⁹ Niku uzani futi kuti, pempani, ndipo muzapasiwa; sakilani, ndipo muzapeza; konkoshani, ndipo bazakusegulilani. ¹⁰ Chifukwa muntu ali onse wamene apempa amalandila; na uja wamene amasakila amapeza; nakuli uja wamene amakonkosha, bazamusegulilako. ¹¹ Nanga nikolo uti pakati panu, wamene ngati mwana amupempa nsomba, azamuoasa njoka mumalo mwa nsomba? ¹² Ngati amupempa sumbi, azamupasa nkanila? ¹³ Mwa ichi, ngati imwe bamene muli boipa muziba kupasa mpaso zabwino kuli bana banu, nanga Tate wanu ali kumwamba si azachilapo apa kupasa Muzimu Oyela kuli baja bamene bamupempa? ¹⁴ Manje Yesu anali kuchosa chibanda chamene sichinali kukamba. Pamene icho chibanda chinachoka, uja mwamuna wamene sanali kukamba anayamba kukamba, nagulu inadabwa. ¹⁵ Koma benangu bantu banakamba kuti, "Kupitila mpavu za Bezebebu, mukulu wa vibanda, akwanisa kutabisa vibanda." ¹⁶ Benangu banamuyesa nakufunisisa chisonyezo kuchokela ku mwamba. ¹⁷ Koma Yesu anaziba maganizo yabo naku bauza kuti, "Ufumu uli onse wamene ugabikana paweka uonongeka, na nyumba yamene igabika ikugwa. ¹⁸ Ngati Satana agabika pa eve eka, nanga ufumu wake uzaimilila bwanji? Chifukwa imwe mukamba kuti ine nichosa vibanda kusebenzesa Bezebebabu. ¹⁹ Ngati ine nichosa vibanda kusebenzesa Bezebebabu, nanga bamene bakukonkani basebenzesa chani? Chifukwa chake, bazankala bokuweluzani. ²⁰ Koma ngati ine nichosa vibanda na kwanja ya Mulungu, ufumu wa Mulungu wabwela pa imwe. ²¹ Ngati mwamuna wampavu wamene ali na vo menyela nkondo vokwanila ayanganila nyumba yake, vintu vake vilibwino, ²² manje ngati wina wampavu amu gonjesa, uja wampavu azatenga vovala vaku nkondo vame uja mwamuna anali kukulupilila naku tenga vintu vonse va uja muntu. ²³ Uja wamene sali naine ashushana naine, nauja wamene sa kolola pamozi naine ataya. ²⁴ Ngati muvi woipa wachoka muli muntu, uma enda kupita mumalo mwamene mulibe manzi kusakila malo yopumulilako. Ngati sunapeze, umakamba kuti, 'Nizabwelela kunyumba kwanga kwamene ninachokela.' ²⁵ Pamene ubwelela, ukapeza ija nyumba niyopyangiwa naku ikiwa mumalo yake. ²⁶ Umayenda naku bwelela pamozi na mizimu zina zili 7 zoipisisa kuichila nakubwela kunkala munyumba ija. Posilizila pake nipakuti uja muntu amankala osila kuchilapo na poyamba." ²⁷ Chinachitika kuti, pamene anali kukamba ivi vintu, mukazi winangu anakwezeka liu yake pa gulu naku kamba kuti, "Niyodala mimba yamene inakubala na mabele yamene yanakunyonsha." ²⁸ Koma anayanka kuti, "Kuchilapo, bodalisika nibaja bamene bamvela mau ya Mulungu naku yasunga." ²⁹ Pamene magulu yanayamba kukula, Yesu anayamba kukamba kuti, "Uyu mubadwe ni mubadwe oipa. Usakila cholangizila, koma kulibe cholangizila chamene chizapasiwa koma cha Yona. ³⁰ Munga mwamene Yona anankalila cholangizila kuli bantu Nineve, chimozi mozi Mwana wa Muntu azankala cholangizila kuli mubadwe uyu. ³¹ Mfumu yayi Kazi yaku mwela izakaima pa siku yoweluza pamozi na bantu ba mubadwe uno naku uweluza, chifukwa eve anabwela kuchokela kosilila ziko kuti amvele nzelu za Solomoni, ndipo onani, mukulu pali Solomoni ali pano. ³² Bantu baku Nineve bazaimilila pa chiweluzo na mubadwe uyu naku wu weluza, chifukwa beve bana tembenuka chifukwa cha kulalika kwa Yona, ndipo onani, mukuli ochila Yona ali pano. ³³ Kulibe muntu, pamene ayasha nyali, ai ika mumalo yobisika kapena pansa pa basiketi, koma poikapo nyali, kuti baja bamene bangena baone ku unika. ³⁴ Linso yanu ni nyali ya thupi. Ngati linso ili bwino, thupi yonse izula na ku unika. Koma ngati linso yanu si ili bwino, thupi yanu izula na mfinzi. ³⁵ Mwa ichi, nkalani osamalila kuti ku unika kwamene kuli mukati mwanu usankale mfinzi. ³⁶ Ngati thupi yanu yonse niyozaza na ku unika, ilibe mbali ili yonse ya mufinzi, thupi yanu yonse izankala munga pamene nyali iwala mofikapo kuli imwe." ³⁷ Pamene anasiliza kukamba, mu Falisi anamupempa kuti ayende akadye kunyumba kwake, Yesu ana enda naku nkala. ³⁸ Mu Falisi anadabwa kuti Yesu sanayambilile kusamba akalibe kudya chakudya chamu mazulo. ³⁹ Koma Ambuye banakamba kuli eve kuti, "Manje apa, imwe ba Falisi mumasuka kunja kwa chomwelamo na mbale, koma mukati muli mozula na kukikonda na voipa. ⁴⁰ Imwe bantu mulibe nzelu! Nanga wamene anapanga kunja siwamene anapanga

namukati? ⁴¹ Pasani kuli bosauka vamene vili mukati, mwamene umu vintu vonse vizankala vokuwamilani imwe. ⁴² "Koma soka kuli imwe ba Falisi, chifukwa mupasa chakumi chavonse vamene mulinavo na volima vamudimba, koma mumakana kuweluza na chikondi cha Mulungu. Ni chofunikila kuchita muchilungamo na kukonda Mulungu, kosa kangiwa kuchita na vinthu vinangu. ⁴³ Soka kwa imwe Afalise, chifukwa mukonda mipando ya kusogolo mu masinagogi na moni waulemu mu malo yogulisila. ⁴⁴ Soka kwa imwe, chifukwa muli monga manda yosalembewapo yemene banthu bayendapo osaziba. ⁴⁵ Umozi wa bakaswili mu malamulo anakamba kuti, "Aphunzisi, vamene mukamba viti tukwana naise." ⁴⁶ Yesu anakamba, "Soka kwa imwe, aphunzisi bama lamul! Chifukwa munyamulisa banthu katundu yoleme yovuta kunyamula, koma imwe simugwilako kutatundu nangu na chukumo chanu chimozi. ⁴⁷ Soka kwa imwe, chifukwa mumanga manda yaba neneli, koma nima kolo yanu yanaba paya. ⁴⁸ Ndimwe mboni na kuvomeleza zinchito zama kolo yanu, chifukwa zoona anabapaya ndipo mumanga manda zao. ⁴⁹ Ndiponso chifukwa chaichi, Mulungu munzeli zake ankamba, 'Nizabatumila baneneli na batumiki, ndipo baza nzunza nakupayapo benengu.' ⁵⁰ Uno mubadwo, ndipo, uzapasiwa mulandu pa magari yonse yabaneneli yana khesewa kuchokela chiyambi cha ziko, ⁵¹ kuyambila magari ya Abelo mpaka magari ya Zakaria, wamene anapaiwa pakati pa guwa na malo oyela. Inde, niku uzani, uno mubadwo uzapasiwa mulandu. ⁵² Soka kwaimwe bakaswili ba lamulo, chifukwa mwatenga chosegulila cha kuziba, imwe bene simungena, ndipo muchingiliza baja bamene bangena." ⁵³ Pamene Yesu anachokako uko, balembe na bafalise banamu susha na kukangana nae pavinthu vambili, ⁵⁴ kuyesa kuti bamugwila mu mau yake.

Chapter 12

¹ Manje, pamene bantu bokwanila ma 1,000 yambili banakumana pamozi mpaka kuyamba kudyakana, anayamba ku uza bopunzila bake choyamba kuti, "munkale bochenjela na chotupisa chaba Falisi, chamene ni umoyo waboza. ² Koma chintu chamene chizabisika chamene sichizazibika. ³ Mwa ichi vamene vikambiwa mu mfinzi chiza onekela poyela, nachamene chikambiwa mu kutu mu chipinda chamukati chiza zibisiwa pamwamba pa malata. ⁴ Nikamba kuli imwe, banzanga, kuti musayope baja bamene bapaya thupi, koma kulibe chinangu chamene bangachite kuchilapo. ⁵ Koma nikuchenjezani pali wamene muyenela kuyopa. Muyope wamene, akapaya, alinayo mpavu kukutayani mu gehena. Zoon, niku uzani, muyopeni. ⁶ Kansi tunyoni tusanu situgulisiwa na ndalama zibili? Koma kulibe nangu kamozi kamene kaibaliwa pa menso ya Mulungu. ⁷ Ngakale na sisi za kumutu kwanu nizopendewa. Musayope. Ndimwe bapa mwamba kuchita tunyoni twambili. ⁸ Ni kamba kuli imwe kuti, ali onse wamene anivomela pamenso pa bantu, Mwana wa Muntu azaka muvomela pamenso pa ba ngelo ba Mulungu, ⁹ koma uja wamene anikana pamenso pa bantu azakakaniwa pamenso pa bangelo ba Mulungu. ¹⁰ Ali onse wamene akamba mau yonyozela Mwana wa Muntu, azakululukiliwa, koma uja wamene anyozela Muzimu Oyela, sazakululukiliwa. ¹¹ Ngati balikuletani kuma Sinagogo, basogoleli, na bolamulila, musankale bovutika mutima mwamene muzazichingizila, kapena vamene muzakamba, ¹² chifukwa Muzimu Oyela uzakupunzisani pantawi yamene iyo vamene muyenela kukamba." ¹³ Pamene apo umozi mugulu ija anakamba kuti, "Apunzisi, mu uzeni mubale wanga agabane naine chuma chamasiye." ¹⁴ Yesu anamuyanka kuti, "Mwamuna, nanga nindani ananipanga oweluzi kapena oimililako iwe?" ¹⁵ Anabauza kuti, "Samalilani kuti muzisunga kutaba vintu vozikonda, chifukwa umoyo wa muntu sunkala mu kupaka kwa vchuma." ¹⁶ Yesu anabauza fanizo, kukamba kuti, "Munda wa muntu olemela inabeleka kwambili, ¹⁷ anaganizila pa eka, kukamba kuti, 'Nanga nizachita chani kansi, chifukwa nilibe malo kosungila vokolola vanga?' ¹⁸ Anakamba kuti, 'Ichi ndiye chamene ine nizachita. Nizagwesa nkokwe zanga naku manga zikulu, mwamene muja nizasungilamo mbeu zanga zonse na katundu. ¹⁹ Nizauza moyo wanga kuti, 'Moyo, iwe uli nacho chuma chamene chasungiliwa cha zaka zambili. Pumula mosavutika, imwa, nkala osangalala.'" ²⁰ Koma Mulungu anamu uza kuti, 'Opusiwa iwe, usiku walelo moyo wako uzatengewa, na vintu vamene wakonzekela, kansi vizankala vabandani?' ²¹ Umu ndiye mwamene muntu wamene azisungila chuma chake koma siolemela pa menso pa Mulungu." ²² Yesu anauza bopunzila bake kui, "Mwa ichi ine nikamba kuli imwe kuti, osaganizila pali umoyo wanu, vamene muzadya; kapena pali thupi, vamene muzavala. ²³ Chifukwa umoyo uchila vakudya, na thupi ichila vovala. ²⁴ Ganizilani vikwangwala, kuti sivishanga kapena kukolola. Vilibe mosungila kapena nkokwe, koma Mulungu amavidyesa. Onani mwamene imwe mupambanilapo kuchila tunyoni! ²⁵ Nanga kansi nindani pali imwe wamene mukupitila movutikila mutima angaikileko ora ku moyo wake? ²⁶ Kansi ngati imwe mukangiwa kuchita kantu aka kang'ono, nanga nichani chamene muvutikila mutima pali vamene vasala? ²⁷ Yanganani pali maluba-mwamene yamelela. Siyasebenza, kapena kutunga vovala. Koma niku uzani imwe kuti, ngakale Solomoni mu ulemelelo wake sana vale vovala monga ivi. ²⁸ Ngati Mulungu akwanisa kuvalika ma uzu yamu munda, yamene yakuti lelo yaliko, koma mailo yataiwa mu mulilo, nikuchilapo kwa bwanji mwamene eve azakuvalikilani imwe, bohepa chikulupililo! ²⁹ Musasakile vamene muzadya na vamene muzamwa, musankale bovutika mutima. ³⁰ Chifukwa maziko yonse ya pa ziko yasakila vintu vamene ivi, ndipo ba Tate banu baziba kuti imwe muvifuna. ³¹ Koma funani ufumu wake, na vintu vonse ivi vizapasiwa kuli imwe. ³² Osayopa, nkosa zochepe, chifukwa ba Tate banu chibamvesa bwino kukupasani ufumu waku mwamba. ³³ Gulisa chuma chako upase kuli bosauka. Zipangile paweka chikwama chamene sichi sili-chuma kumwamba chamene sichisila, kwamene kulibe kawalala wamene abwela pafupi, kapena zimbili kuononga. ³⁴ Chifukwa kwamene kuli chma chako ndiye kwamene kuli mutima wako. ³⁵ "Nkalani bokonzekela na nyali zanu zikanzinkala zoyaka, ³⁶ ndipo munkale monga bantu bamene bwana wabo pamene abwelela kuchoka ku pwando ya ukwati, kuti pamene abwela kukonkosha, mosachedwa bazamu segulilako. ³⁷ Bodalisika nibaja bantchito bamene bwana wabo azabapeza balanganila pamene abwelela. Zoon, niku uzani kuti, azakonzekelatatu naku baitana kuti bankale podyela, ndipo azabwela naku batumikila. ³⁸ Ngati bwana abwela pa ntawi ya chibili ya usiku, kapena yachitatu, naku bapeza bali bokonzekela, nibo bodalisika bantchito abo. ³⁹ Koma mvesesani ichi, asemble mwine wa nyumba anaziba ntawi yamene kawalala azabwela, sangalekelele nyumba yake kuti angenemo. ⁴⁰ Naimwe nkalani bokonzekela, chifukwa simuziba ntawi yamene Mwana wa Muntu azabwela." ⁴¹ Petulo anakamba kuti, "Ambuye, nanga mukamba iyi fanizo ku uza ise chabe, kapena kuli bonse?" ⁴² Ambuye banamuyanka kuti, "Nanga kansi niuti okululupilika futi wanzelu olanganila wamene mbuye wake azaika kuti apase mbali yao yacha kudya pa ntawi yake yoenela? ⁴³ Odalisika ni uja wantchito wamene mbuye wake amupeza achita chamene ichi pamene abwela. ⁴⁴ Zoon niku uzani kuti azamu kwezeka kunkala olanganilka katundu wake wonse. ⁴⁵ Koma ngati uja wantchito azakamba mumutima wake kuti,

'Mbuye wanga achedw kubwelela,'nakuyamba kumenya bantchito bamuna na bakazi nakuyamba kudya nakukolewa,⁴⁶ mbuye wauja wantchito azakabwela pa ntawi yamene sazayembekela na pa ola yamene sazaziba naku mujuba mu vidunswa vidunswa naku mugabila malo pamozi nabaja bosakululupilika.⁴⁷ Uja wantchito, wamene anaziba chofuna cha bwana wake koma sanakonzekela kapena kuchita kulingana na chofuna chake, azamenyewa na kwambili.⁴⁸ Koma uja wamene sanazibe koma anachita chamene chofunikila kumenyewa, azamenyewa pangóno. Koma ali onse wamene anapasiwa vambili, kuli beve vambili vizafunsiwa, nauja wamene anali ana pasiwa vambili, vambili vizanfusiwa kuli eve.⁴⁹ "Nina bwela kutila mulilo paziko, ningafunisise kuti unali oyaka kudala."⁵⁰ Koma nili nao ubatizo wamene nifunika kubatiziwa nao, ndipo mwamene nili ovutika mpaka chifikiliziwe!⁵¹ Nanga muganiza kuti ine ninabwela kuleta mutendere pa ziko? Iyayi, Niku uzani imwe, koma kugabikana.⁵² Chifukwa kuchokela apa kuzankala basanu munyumba imozi bogabikana-batatu kushushana na babili, na babili kushushana na batatu.⁵³ Bazankala bogabikana, tate kushusha mwana na mwana kushusha tate, muzimai kushusha mwana na mwana kushusha mai, mupongozi-mukazi kushusha mupongozi mukazi na mupongozi mukazi kushusha mai mupongozi."⁵⁴ Yesu anali ku uza magulu nafuti kuti, "Ngati mwaona kumbi i'ima kuchokela kumazulo, pamene apo mumakamba kuti, 'Mvula ingóno ibwela.' chimachitika munjila yamene iyo."⁵⁵ Ngati chimpepo chochokela kumwela chitimba, mumakamba kuti, 'kuzapya maningi,' ndipo chimachitika.⁵⁶ Baboza, muzima tantauzo ya ziko na makumbi, nanga bwanji imwe simuziba tantauzo ya ntawi yamanje?⁵⁷ Nanga kansi nichifukwa chani imwe simukwanisa kuweluza cholungama pa imwe mweka?⁵⁸ Chifukwa ngati imwe muyenda na mudani wanu ku oweluza milandu, munjila yesesani kuti mukambilane mulandu uyo kuti asakupelekeni kuli oweluza, mwakuti oweluza asakupelekeni kuli kazembe, na kazembe asakupelekeni mundende.⁵⁹ Niku uzani imwe kuti, simuzakachoka mundende mpaka mukasilize kulipila ndalama zonse."

Chapter 13

¹ Pa ntau ija, bantu benangu kuja ba namu-uza pali baku Galileya bamene Pilato anasanganiza magazi yabo na nsembe. ² Yesu anayanka na kukamba kuli benve, "Muganiza kuti aba baku Galiley banali bochimwa Maningi ku chila bamu Galileya bonse chifukea bana vutika munjila iyi?" ³ Iyai, niku uzani. Koma ngati simutembenuka, monse muza onogeka munjila imozi. ⁴ Olo baja bantu bali 18 mu Siloamu banagwelewa na nyumba yapamwamba naku bapaya, Muganiza kuti baanali bochimwa maningi kuchila bantu bonse mu Yelusalema? ⁵ Iyai, Nikamba. Koma ngati simutembenuka, monse muza onogeka." ⁶ Yesu anakamba fanizo iyi, "Muntu winangu anali na Mutengo wampesa woshangiwa mumunda wake na mpesa anabwela kusakila vipaso mu mutengo koma sana vipeze. ⁷ Muntu ana uza bolima mmuunda, "Ona, zaka zitatu manje nibwela na kuyesa kupeza vipaso pa mutengo wampesa uyu koma sini na peze chii chonse. Chijube. Nanga nichani kuchilekelela ku ononga ntaka?" ⁸ "Olima mu munda anayanka naku kamba kuti, 'Chisiyeni chka chino pamene ni limila mumbalu mwake na kuyikamo manyowa. ⁹ Ngati chaba vipaso chaka chibwela, chabwino; koma ngati sichina bale, uchi jube!" ¹⁰ Manje Yesu enze ounzisa mu sinagogo inangu ntawi ya Sabata. ¹¹ Onani, panali muzimai enze na muzimu woipa kwa zaka 18. Enzo obenda musana senzo kwanisa kuyondoloka maningi. ¹² Pamene Yesu ana muona, anamuitana naku kamba kuti, "muzimai, wamasuliwa kumatenda yako." ¹³ Anaika manja yake pali enve, ndipo pamene apo anayondoloka na kupasa Mulungu ulemelo. ¹⁴ Koma musogoleli wa sinagogo anakalipa chifukwa Yesu anapolesa pa Sabata ndipo musogoleli anakamba kuli gulu, "Muli masiku yali 6 yamene yali yofunkaila kusebenza. Bwelani mu polesewe kansi, osati pa siku ya Sabata." ¹⁵ Ambuye anamuyanka kuti, "Ba chinyengo! imwe monse simuma mangusula ng'ombe zanu kapena bulu kuchoka mukola nakuzi peleka kumwa manzi pa Sabata?" ¹⁶ Chimozi mozi na uyu mwana mukazi wa Abrahamu, wamene Satana ana manga kwa zaka zambili zokwana 18, sembe kumangiwa kwake sikuna mangusuliwe pa siku ya Sabata?" ¹⁷ Pamene enzo kamba ivi vintu, bonse benzo mu ukila banamvela, koma gulu yonse inali kusangalala pali vintu vonse va ulemelelo vamene anachita. ¹⁸ Pamene apo Yesu anakamba kuti, "Ufumu wamulungu uli monga chani, elo ninga ulinganize nichani?" ¹⁹ Uli monga ka mbeu ka mupilu kamene muntu anatenga nakuka ponyela mumunda mwake, ndipo ina kula kunkala chimutengo chikulu, na nyoni zamu mwamba zina manga tunchisa twake mu mwama mwake," ²⁰ Anakamba futi, Nichani chamene ninga linganize ufumu wa Mulungu?" ²¹ Uli minga chofufumisa mukate chamene muzimai anatenga naku sankaniza na unga wa mukate okwanila mupimo utatu mpaka china mwazyika mu unga wa mukate onse." ²² Anabwela Yesu anayenda kupita mumizinda na munzi, kupunzisa na kupanga njila yake yoyenda ku Yelusalema. ²³ Muntu wina anakamba kuli enve, "Ambuye, Ninshi nibantu bang'ono chabe baza pulumusiwa?" Abwela akamba kuli enve, ²⁴ "Lwishani ku ngena mukaseko kang'ono, chifukwa nikamba kuli iwe, bambili bazayesa ku ngena, koma sibaza kwanisa kungena. ²⁵ Chabe mwine wa nyumba aka nyuka na kukoma chiseko, Ninshi uza ilimila panja naku menya chiseko nakukamba, 'Ambuye, Ambuye, tingeneseni.' "azayanka nakukamba kuli iwe, 'Sini kuziba olo kwamene uchokela.' ²⁶ "Koma uza kamba, 'tinadya na kumwa pa menso pako elo una punzisa mu njila zatu. ²⁷ "Koma aza yanka, "Nikamba kuli imwe, siniziba kwamene mu chokela. chokani pali ine, imwe bamene muchita uchimo!" ²⁸ Kuzankala kulila na kukokota meno mukaona Abrahamu, Isaki, Yakobo, na bonse baneneli mu ufumu wa Mulungu, koma mwa ponyewa panja. ²⁹ Baza choka kumaba, kumazulo, kumpoto na kumwela, na kunkala pa ome mu ufumu wa Mulungu. ³⁰ Zibani ivi, abo basiliza baza nkala boyamba, na abo bofunikila bazankala bosiliza." ³¹ Mu ntau yamen ija, afalisi benanfo bana bwela nakukamba kuli enve, "yendani naku choka apa chifukwa Heoda afuna ku kupaya." ³² Yesu anakamba kuti, "Yendani mukayi uze nkandwe ija, 'onani ni chosa madimoni na kupolesa lelo na mailo, na siku ya chitatu nizafika pamene nifuna kufika.' ³³ Ngati si ivo, nicho funikila kuti ni pililize lelo, mailo, siku yo konkapo, pakati si chovomelezewa kuti muneneli awonongewe panja pa Yelusalema. ³⁴ Yelusalema, Yelusalema, wamene apaya baneneli na myala abo botumiwa kuli imwe. mwanene nenzo funisisila ku sonkanisa bana bako monga mwamene nkuku imasonkanisila tubana twake pansu pa mapapiko yake, koma simuna funisise ichi. ³⁵ Ona, nyuma yako ya siyiwa. nikamba kuli iwe, si uzani ona mpaka ukambe, 'wodaliska ni wamene abwela muzina ya Ambuye.'"

Chapter 14

¹ Chinachitika sabata imozi, pamene nanangena mu nyumba ya musogolelei umozi wa bafalise kuti adye buledi, banali kumu yanganisisa. ² Onani, pasogolo pake panali mwamuna wamene enzeli kunzunzika na matenda yovimbisa manja na mendo. ³ Yesu anafunsa bakaswili ba lamulo yaba Yuda na ba Falise, "Nishoyenela kuchilisa pa Sabata, nagu iyai." ⁴ Koma bana nkhal zii. Mwaicho Yesu anamugwila, kumuchilisa, naku mu uza ayende. ⁵ Anabauza, "Nindani pali imwe ali namwana mwamuna, nagu ngombe yamene yagwela mumgodi pa siku ya Sabata sangamumchose pamene apo?" ⁶ Sibana kwanise kupasa yankho kuli ivi vinthu. ⁷ Pamene Yesu anaona mwamene baja bamene banaitaniwa benzeli kusankhila mipando yolemekezeka, anakamba fanizo, kubauza kuti, ⁸ "Pamene uitaniwa na nawinangu kuphwando ya ukwati, usankhale pa malo yolemekezeka, chifukwa kapene baitana winangu wolemekezeka kupambana iwe. ⁹ Pamene munthu wamene akuitanini bonse babili afika, azakuuza, 'Pasa uyu munthu malo yako,' ndipo na nsoni uzayenda nakutenga malo yakosilizila. ¹⁰ Koma bakakuitana, yenda na kunkhala pamalo yakosilizila, kuti pamene wamene akuitana abwela, angaku uze kuti, 'Munzanga, yenda pamwaba.' Ndipo uza lemekezika pamenso pa bonse beli nkhal pa thebo naiwe. ¹¹ Chifukwa alionse wamene azikweza azachepesewa, ndipo wamene azichepesa azakwezewa." ¹² Yesu anauza futi mwamuna wamene anamuitana, "Pamene upasa chakudya cha mumazulo kapena phwando, osaitana banzako kapena babale bako kapena babululu bako kapena bapafupi bo;lemela, chifukwa naiwe banga kuitane kubwezele ndipo uzabwezelewa malipilo. ¹³ Koma ukapasa phwando, itana osauka, opunduka, olemala, na osayangana, ¹⁴ ndipo uzadaliska, chifukwa sibanga kumbwezele malipilo. Chifukwa uzalipiliwa mu kuukisiwa kwa olungama ¹⁵ Pamene umozi wa bamene bankhala na Yesu pathebo anamvela ivi vinthu, namuza kuti, "Odaliska ni uyo wamene azadya buledi mu ufumu wa Mulungu!" ¹⁶ Koma Yesu anamu uza kuti, "Munthu winangu anakonzekela chakudya chamumazulo chikulu nakuitana bambili. ¹⁷ Pemene chakudya chamumazulo china konzekewa, anatuma banchito bake kuti auze bemene bana itaniwa, 'Bwelani, chifukwa vonse vakonzekewa.' ¹⁸ Bonse banyamba kupa madandaulo. Oyambila anamu uza, 'Nagula munda, nifunika niyende niuwone. nipempha munikhululukile.' " ¹⁹ Winangu anakamba, 'Nagula ngombe zolimila magulu 5, ndipo niyenda kuziyesa. Nipempha munikhululukile.' ²⁰ "Winangu anakamba kuti 'Nakwatila mukazi, ndipo chifukwa chaichi siniga bwele.' ²¹ "Wanchito anabwela naku uza bwana wake ivi vinthu. Ndipo bwana wanyumba anakalipa naku uza wanchito wake, 'Yenda musanga mumisao ya muzinda na kuleta osauka, opunduka, osayangana, na olemala.' ²² "Wanchito anakamba kuti, 'Bwana, vame mwalamulila vachitiwa, koma malo yakaliko. ²³ "Bwana anauza wanchito, 'Yenda mumiseo yonse kunja kwa muzinda, ubakaka babwele, kuti nyumba yanga izule. ²⁴ Chifukwa niku uza, palibe pali aba banthu bamene banaitaniwa wamene azalba chakudya changa chamumazulo." ²⁵ Manje magulu yakulu yenzeli kuyenda naye, ndipo anapindamuka naku bauza, ²⁶ "Ngati alionse abwela kuli ine ndipo sazonda batate bake, bamai bake, bana bake, babale bake naba longosi, naumoyo wake, sanga nkhal ophunzila wanga. ²⁷ Alonse wamene sanyamula mutanda wake na kunikonkha sangankhale ophunzila wanga. ²⁸ Nilndani pali imwe wamene afuna kumanga nyumba itali sayambila kunkhala pansi naku penda kuti aone ngati ali navo vofunikila kuti aisilize. ²⁹ Ndaba, ngati aika maziko naku kangiwa kulsiliza, bonse boona bazayamba kumunyoza, ³⁰ kukamba kuti, 'Uyu munthu anayamba kumanga koma anakangiwa kusiliza.' ³¹ Nagu nimfumu yabwanji, pamene ayenda kukumana na mfumu inangu mu nkondo, siyambila kunkhala pansi kuti itenge nzelu kuona kuti ngati angende na banthu bake 10 000 kuti amenyane na mfumu inagu ili na banthu 20 000? ³² Ngati sanga kwanise, pamene gulu inangu yankhondo ikali kutali, atuma nthumi naku funsa vofunukila kuti pankhale mutendele. ³³ Mwaicho, alionse wamene sasiya vonse nakunikonkha sanga nkhal ophunzila wanga ³⁴ Sauti niyabwino, koma ngati sauti yaleka kumveka monga sauti, ingapangiwe bwanji sauti futi? ³⁵ Siinga sebenzesewe kuli chili chonse. Utaiwa. Wamene ali na matu, lekani amvele.

Chapter 15

¹ Mwaichi bonse bokomesa musonko na bochimwa banali kubwela kuli Yesu ku mvela kuli enve. ² Pamozi ba Falisi nabo lemba banayamba ku kambila mumutima kukamaba kuti, "Uyu muntu alandila ba chimwa, kudya nabo." ³ Yesu anabauza mwambi kukamba kuti, ⁴ "Ni ndani pali imwe, ngati ali nambelele zili 100 ndipo asobesapo imozi, sanga siye zili 99 mu chipululu nakuyendakusakila ya soba mpka ayi peza?" ⁵ Ngati ayipeza, ayike pama pewa naku kondwela. ⁶ Pamene afika ku nyumba, ayitana banzake naba nansi bake, nakukamba kuli benve, 'sangalalani pamozi naine, chifukwa napeza mbelele yanga ina soba.' ⁷ Ni kamaba kuli imwe kuti olo apo, ku zankala kukondwela kumwamba ngati wochimwa umozi atembenuka, kuchila bopitilia 99 bolungama bamene sibafuna kutembenuka. ⁸ Olo ni mukazi bwanji ali nandalama za siliva 10, ngati asobesapo imozi, sanga yashe nyali, nakupyanaga munyumba, na kusakila bwino mpaka ayipeza? ⁹ Pamene ayi peza, azaitana banzake naba nansi bake, sangalalani naine, chifukwa naipeza ndalama tanga ina soba. ¹⁰ Ngakale ivo, niku uzani, kuli chisangalalo pamenso pabangelo bamulungu pali umozi ochimwa atembenuka. ¹¹ Ndipo Yesu anati, "Muntu wina anali na bana bamuna babili, ¹² ndipo mungono pali benve anakamba kuli batate bake, Batate nipasenkonni mbali ya chuma changa." Mwaicho anaba gabanisa katundu yake pakati. ¹³ Pakalibe kupita masiku yambili, mwamuna mungono anaika pamozi vamene vinali vake nakuyenda ku ziko yakutali, ndipo kuja anaononga chonse chuma chake pakunkala osakilako nzelu. ¹⁴ Pamene anasiliza vonse, njala ikulu inankalako mu chalo chija, ndipo anayamba kuvutika. ¹⁵ Anayenda nakupeza nchito kul umozi pa bonkala muziko ija, wamene ana mutuma mu malo yake ku dyesela nkumba. ¹⁶ Anayamba kudya vosalapo vamene nkumba zinali kudya chifykwa palibe anali kumupasa chili chonse. ¹⁷ Pamene mwana mungono anaganiza pa eka, anakamba, niba ngati pa banchito ba batate banga bamene bali nawa mbili mukate, ndipo nili kuno, nikufa nanjala! ¹⁸ Nizanyamuka naku chokako kuno nakuyenda kuli batate banga, ndipo nizabauza kuti, "Tate, na chimwila kumwamaba nakuli imwe." ¹⁹ Siniyela kuitaniwa mwana wanu, nipangeni chabe monga umozi pa banchito banu." ²⁰ Mwana mungono uja anayamuka nakuyenda kuli batate bake. pamene anali patali maningi, batate bake bana muona, bana mvela chifundo, ndipo bana mutamangila nakumu kumbatila baku mu pyopona. ²¹ Mwana anabauza, "Batate, nachimwa kumwamba akuli imwe, sindine oyenelela ku itaniwa mwana wanu." ²² "Batate bake anauza ba nchito babo, letani musanga chovala chabwino, nakumuvalika, naku muvalika mpete kukwanja kwake, na nsapato kumendo kwake. ²³ Letani ngombe yoina nakuyi paya. Lekani tipange pwando nakukondwela! ²⁴ pakuti mwana wanga anali anafa, manje ali moyo. Anali anasoba, koma manje apezeka, mwaicho bana yamba kusangalala. ²⁵ "Manje mwana wake mukulu anali ku munda. Pamene anabwela na kufika panyumba, ana mvela nyimbo nakuvina. ²⁶ Anaitana umozi waba nchito nakumufunsa nanga nivi chani. ²⁷ Wanchito anakamba kuli enve, "Mubale wako abwela panyumba ndipo batate bakonbamupaila, ngombe yoina chifukwa ba mulandila bwino." ²⁸ "Mwana mukulu anakalipa sana fune na kungena mukati, ndipo batate bake bana choka panja nakuyamba kumupapata. ²⁹ Koma mwana mukulu anayanka naku kamaba kuli batate bake, 'Onani, zaka zambili nina kusebenzelani, ndipo sinina kanepo lamulo yanu, ndipo simuna nipaseko kamwana kambuzi kuti nikondwele naba zanga. ³⁰ Koma pamene mwana wanu anabwela, Wamene andya chuma chanu nama hule, mwamu payila mwana wangombe yoyina.' ³¹ "Batate bake banamu uza kuti, 'Mwana, iwe umankala naine ntawi zonse, na vonse vanga nivako. ³² Koma chinali cha bwino kuti tikondwele na kusangalala, chifukwa mubale wami anali qa kufa manje alimoyo; enze anasoba koma manje apezeka.'"

Chapter 16

¹ Yesu naenve anakamba kuli bopunzila bake, "Kunanili mwamuna olemela wamene anali na olanganila ndipo china nenelewa kuli benve kuti olanganila wake ² anali ku ononga vintu vake. Mwaichi mwamuna olemela ana muitana naku kamba kuli enve, "Nivi chani ivi vamene nimvela oali iwe? kamba pa vintu vamene wa sebenzelapo chifukwa suza nkala oyanganila." ³ "Olanganila anakamba kuli eka, "Nizachita chani pakuti mbuye wanga atenge nchito yanga yo yanganila? Nilibe mpavu yonkumbila, ndipo nina nsoni kupempa. ⁴ Niziba vamene niza chita, chakuti ngati pamene niza chosewapo pa chinto yanga yo yanganila, bantu baza ni landila muma nyumba yabo." ⁵ Mwaicho ologaninila anaitana aliyense umozi anali nankongole ya mbuye wake, naku funsa oyamba una nkongole zingati za mbuye wanga? ⁶ "Anakamba kuti, 'Tenga 100 mumafuta ya oliva. 'Anakamba kuli enve, 'Tenga zolipila zako nkala pansi mwamusanga naku lemba 50.' ⁷ "Mwaicho olanginila anakamba kulu muzake 'Nkongole yako nizingati?' "Anakamba mipimo 100 ya tiligu.' Anakamba kuli enve, 'Tenga zolipila zako, naku lemba 80.' ⁸ Mbuye wake analamulila oyanganila osalungulama chifukwa anachita mochenjelesa. Chifukwa bana bamu chalo bachita mochenjela kuli bantu babo ku chila bantu balimunyali. ⁹ Ni kamba kuli iwe, zipangile banazako na ndalama chilibe chilungamo kuti chikasila, banga kulandile mu malo ya muyayaya. ¹⁰ Wamene ali okululupilika muka mukang'ono niokulupilikanso namu vambili, na wamene alibe chilungamo mu vambili. ¹¹ Ngati siwene okulupilika muku sebenzesa ndalama chosa lungama, nindani azakulupililana chuma cha zo-ona? ¹² Ngati sibenze bokulupilika mukusebenzesa katundu ya bantu, nindani azakupasa ndalama zako? ¹³ Kulibe wanchito anga sebenzele ba mbuye babili, chifukwa azazonda winangu naku konda winangu, olo kapena azankala oziipeleka kuli umozi naku sula winangu. Sungatumikile Mulungu na ndalama." ¹⁴ Manje Afilisi, benzeli bokonda ndalama, bananvela vonse ivi vintu, bana museka. ¹⁵ Anakamba kuli benve, "Muzilungamisa pamenso ya bantu, koma Mulungu aziba mutima yanu. chiya chamene nichokwezekewa pakati pa bantu nicha nsoni mumebso yamulungu. ¹⁶ Lamulo naba nenli banali bosatili kufikila pa ntawi yamene Yohani anabwela. kuchoka pa ntawi ija, uenga wabwino wau ufumu wa Mulungu ulaliki; bonse bafuna kuzipatikiza kungenamo. ¹⁷ Koma sichovuta kuti kumwamba na ziko ya pansi kupita kupambana kalemba kamozi kalamulo kunkala kalibe nchito. ¹⁸ Aliyense wamene asiliza chikwati namukazi wake naku kwatila winangu achita chigololo ndipo wamene akwatila mukazi wamene chikwati chinsula na mwamuna wake achita chigololo. ¹⁹ "Manje kunali mwamuna winangu otemela wamene anavala vovala va mpepo na nyula ya bwino siku iliyonse na ndalama chake chambili. ²⁰ Panali opempa winangu zina yake Lazalo enzeli ogonekewa pongenela pake na vilonda tupi yake yonse, ²¹ ndipo anali kufunisisa kudya vamene vinali kugwa kuchokela pa tebulo yabolemela. Namaimbwa yanali kubwela kumyanguta vilonda vake. ²² Ntawi inabwela pamene opeme[a anafa ndipo ananyamuliwa nabangelo kumbali ya Abrahamu. Mwamuna olemela naye anafa naku shikiwa, ²³ ndipo mu Hadesi, kunkala ozunziwa, ananyamula menso yake kumwamba anaona Abrahamu kutali na Lazalo pambali pake. ²⁴ Mwaichi analila naku kamba kuti, 'tate Abrahamu, ninveleni chifundo mutumeko Lazalo, kuti angenese kakumo mu manzi naku zizilika lulimi yanga, nichifukwa nili naukali mu mulilo umu. ²⁵ "Koma Abrahamu anakamba, 'Mwana, kumbukila mu ntawi yako yau muuo unaladila vabwino vako ndipo Lazalo mu vintu monga voipa. koma manje niolibisiwa kuno, ndipo ndiwe ²⁶ opwetekewa. Olo kuti nichoncho, paikiwa chimugodi chikulu pakati bamene bafuna kutauka kuchoka uko sibanga kwanise, ndipo kuchokela kuli ise.' ²⁷ "Mwamuna olemela anakamba, 'Niku pempani, Tate Abrahamu, kuti ungamuteme kuli nyumba ya batate banga- ²⁸ chifukwa nili naba kalongosi bali 5- kuti angaba chenjeze, chakuti basaka bwele mu malo yo vutisiwa. ²⁹ "Koma Abrahamu anakamba, 'Bali na Mose na baneneli, leka bamvelele benve.' ³⁰ "Mwamua olemela anayanka, 'Iyai Tate Abrahamu, koma ngati muntu anga yende kuli benve kuchoka ku boukufa, bazalapa.' ³¹ "Koma Abrahamu anakamba kuli benve, 'Ngati sibazamvelela aukisiwa ku boukufa sibazaba mvela.'"

Chapter 17

¹ Yesu anauza bopunzila bake kuti, "Nichosimikizika kuti kuzankala vintu vamene vingalese kuti ise tichimwe, koma soka kuli uja wamene vipitila!" ² Chawamapo kuti chimwala chotwelapo chimangiwe kumukosi kwake nakumutaya mu nyanja kuchila kuti alengese umozi mwa aba bana kuti bagwe. ³ Zilanganeni pamweka. Ngati mubale wako achimwa, mukalipile, ngati atembenuka mukululukile. ⁴ Ngati akuchimwila iwe kokwana 7 musiku imozi, koma abwela futi kali 7 kuli iwe, kukamba kuti, 'Nalapa,' uyenela kumukululukila!" ⁵ Batumiki bana uza Ambuye kuti, "Tikuliseni chikululupilo." Ambuye banabayanka kuti, "Imwe asembe munali nacho chikulupililo monga kambeu ka mpiru, ⁶ asembe mukamba kuli uyu mutengo wa mukuyu kuti, 'Zinyule, enda kazishange mu nyanja,' ndipo chizakumvelelani imwe. ⁷ Koma ni uti pakati kanu, wamene ali nao wantchito wamene alima kapena kulanganila mberere, azamu uza akachoka ku munda kuti, 'Endesa manje manje ubwela unkale udye?' ⁸ Nanga sazamu uza kuti, 'Nikonzele chakudya ine nidye, vala vovala voyenela ubwele uni tumikile mpaka nisilize kudya nakumwa. Kuchoka apo manje iwe ungadye nakumwa?' ⁹ Sazamuyamika wantchito uja chifukwa achita ntchito yamene bamu uza, nanga amachita icho? ¹⁰ Chimozi mozi naimwe, ngati mwachita chintu chamene mwauziwa, muyenela kukamba kuti, 'Ise ndiye bantchito bamene siboyenela. Tachita chabe vamene tiyenekela kuchita. ¹¹ Pamene eve anali kuyenda ku Yelusalem, anapitila ku malile ya pakati pa Samaliya na Galileya. ¹² Pamene anangena mu munzi umozi, anakumana na bantu kumi bamene banali bamakate. Banaimilila kutali ¹³ na eve naku kwezeka liu yabo, kukamba kuti, 'Yesu, Kazembe, tichitleni chifundo ise.' ¹⁴ Pamene anaba ona eve, anabauza kuti, 'Endani mukazionese kuli wansembe.' Pamene banali kuyenda bana polesewa. ¹⁵ Pamene umozi pali beve anaona kuli apola, anabwelela, mopunda ndishi alemekeza Mulungu. ¹⁶ Anagwa pansi pa mendo ya Yesu kumuyamika. Anali mu Samaliya. ¹⁷ Yesu anakamba kuti, 'Kansi aba sibanal kumi bamene banapolesewa? Nanga benangu bali 9 bali kuti? ¹⁸ Kansi kulibe benangu bamene babwelela kupeleka ulemelelo kuli Mulungu, koma uyu chabe mukunja?' ¹⁹ Anamu uza kuti, 'Imilila, uyende. Chikulupililo chako chakupolesa.' ²⁰ Pamene anafunsiwa na ba Falisi pamene ufumu wa Mulungu uzakabwela, Yesu anabayanka kuti, 'Ufumu wa Mulungu siumabwela na kulanganisisa. ²¹ Sibazakakamba kuti, 'Onani, uyu apa'" kapena kuti, 'Uyo kuja!' Chifukwa onani, ufumu wa Mulungu uli mukati mwanu." ²² Anakamba kuli bopunzila bake kuti, 'Masiku yazabwela pamene muzakafunisisa kuona siku imozi ya Mwana wa Muntu, koma simuza kaiona. ²³ Bazakabwela baka ku uzeni kuti, 'Onani, kuja! Onani, uku!' Koma musabakonke kapena kubatamangila, chifukwa ²⁴ mwamene kaleza kamasanikila kuchokela kakayaka kumalo kumoji kumwamba mpaka kumbali yina yaku mwamba, chimozi mozi Mwana wa Muntu azakankalila pa ntawi yake. ²⁵ Koma poyamba ayenela kuvutika mu vintu vambili naku kaniwa na mubadwe uno. ²⁶ Monga mwamene china chitikila mu ntawi ya Nowa, ndiye mwamene chizakachitikila mu ntawi za Mwana wa Muntu. ²⁷ Banadya, banamwa, banakwatila, nakupelekewa ku chikwati kufikila ntawi yamene Nowa anangena mu bwato-na chigumula chinabwela naku baononga bonse. ²⁸ Chimozi mozi, monga mwamene chinachitikila mu ntawi ya Loti-banali kudya na kumwa, kugula na kugulisa, kushanga na kumanga. ²⁹ Koma pa siku yamene Loti anachokamo mu Sodoma, kunalokwa mulilo na Salifa kuchokela ku mwamba naku baononga bonse. ³⁰ Munjila imozi mozi ndiye mwamene chizankalila pa siku yamene Mwana wa Muntu azakaonekela. ³¹ Pa siku ija musakamuleke wamene ali pamalata kuti ayende pansi kuti akatengge katundu wake munyumba, nauja wamene ali ku munda musamu vomelese kuti abwelele. ³² Kumbukilani mukazi wa Loti. ³³ Uja wamene afunisisa kuti asunge moyo wake azautaya, koma wamene ataya moyo wake azaupulumusa. ³⁴ Niku uzani imwe kuti, pa usiku uja kuzakankala bantu babili pogonela. Umozi azakatengewa, winangu azaka si iwa. ³⁵ Kuzakankala bakazi babili bakutwa pamozi. Umozi azakatengewa, winangu azakasi iwa." ³⁶ Kuzakankala bantu babili mu munda; umozi azakatengewa winangu azaka si iwa." ³⁷ Banamufunsa kuti, "Kuti, Mbuye?" Anaba yanka kuti, ! Kwamene kuli tupi, ndiye kwamene vi kwalala viza kaunjikana."

Chapter 18

¹ Anabwela abauza fanizo beve kubalangiza kuti bayenela kunkala bopempela ntawi yonse osati bobwezewa kumbuyo, ² kukamba kuti, "Mu muzinda wina munali muweluzi uyo wamene sanali kuyopa Mulungu kapena kupasa ulemu bantu. ³ Manje munali ofewa mumuzinda wamene uyo, anali kubwela kuli eve kambili, kukamba kuti, 'Nitandizeni kutenga chiweluzo na oshushana naine.' ⁴ Kwa ntawi yambili sanali kufuna kumutandizila, koma pamene panapitako ntawi anazi uza kuti, 'Ngakale kuti ine sinoyopa Mulungu kapena kulemekeza muntu, ⁵ manje chifukwa chakuti uyu ofewa anivuta, nizamutandiza kuti atenge chiweluzo, mwakuti asani lemese chifukwa chobwela bwela.'" ⁶ Ambuye banakamba kuti, "Mvelani vamene muweluzi wamene alibe chilungamo akamba. ⁷ Manje nanga Mulungu sazabwelesa chiweluzo kuli baja bamene bama lila kuli eve usiku na muzuba? Nanga azachedwa kubalanga napo? ⁸ Niku uzani kuti azabaletela chiweluzo musanga. Chimozi mozi, pamene Mwana wa Muntu azakabwela, nanga azaka pezapo chikulupililo pa ziko?" ⁹ Anakamba nafuti iyi fanizo kuli benangu bamene banali bozilimbikisa mukati mwabo kuti banali bolungama naku sula bantu benangu, ¹⁰ "Bamuna babili bana enda mu tempele kukapempela-umozi anali mu Falisi na winangu wa misonko. ¹¹ Mu Falisi anaimilila naku pempela vintu ivi pali eve, 'Mulungu, niku yamikani kuti ine sinili monga bantu benangu-mbava, balibe chilungamo, bachigololo-kapena monga nauyu wamisonko. ¹² Ine nimazimana chakudya kabili mu sabata. Nimapasa chakumi pa vonse vamene nimalandila. ¹³ 'Koma uja wamisonko, ali imilile patali, sana imye na menso yake kumwamba, koma anali kumenya pa chifuba chake, kukamba kuti, 'Mulungu, nichitleni chifundo ine, muntu wamachimo. ¹⁴ 'Niku uzani kuti, uyu muntu anayenda kunyumba kwake olungamisiwa kuchila uja winangu, chifukwa muntu ali onse wamene azikwezeka azabwezewa, koma ali onse wamene azichepesa azakwezewa." ¹⁵ Bantu banali kumuletela bana bangono kuti abaikepo kwanja, koma pamene bopunzila bake banaona ichi, banaba kalipila. ¹⁶ Koma Yesu anabaitana, kubauza kuti, "Balekeni bana bangono kuti babwele kuli ine, musabalese. Chifukwa ufumu wa Mulungu niwa bantu bamutundu uyu. ¹⁷ Zoona niku uzani kuti, ali onse wamene saza landila ufumu wa Mulungu monga kamwana nichosimikizika kuti saza ungenamo." ¹⁸ Wina olamulila anamufunsa funso, kukamba kuti, "Mupunzisi wabwino, nanga nichani chamene niyenela kuchita kuti ine ninkale namoyo wamene siusila? ¹⁹ Yesu anamuyanka kuti, "Nanga nichani chamene uni itanila kuti ndine wabwino? Kulibe wabwino, koma Mulungu chabe. ²⁰ Uyaziba malamulo-Osachite chigololo, usapaye, osabe, osapase umboni waboza, lemekeza batate na bamai bako." ²¹ Olamulila anamuyanka kuti, "Vonse ivi nimavichita kuchokela pamene ine ninali mungono." ²² Pamene Yesu anamvela ivi, anamu uza kuti, "Kulibe chabe chintu chimozi chamene upelebela. Uyenela kuyenda kugulisa vintu vako vonse naku pasa bantu bosauka, uzankala na chuma kuwamba-ubwele, unikonke ine." ²³ Koma pamene uja olamulila anamvela ivi vintu, anamvesana chifundo, chifukwa anali olemela maningi. ²⁴ Pamene Yesu, anamuona kuti amvesana chifundo ana kamba kuti, "Onani mwamene chilili chovuta kubaja bamene bali na chuma kuti bangene mu ufumu wa Mulungu! ²⁵ Nichapa fupi kuti kavalo ingene mukamu bo ka nyeleti, kuchilapo muntu olemela kuti angene ufumu wa Mulungu." ²⁶ Baja bamene ba mvelako banakamba kuti, "Kansi nanga nindani wamene angapulumuke?" ²⁷ Yesu anabayanka kuti, "Vintu vamene vili vovuta kuli bantu nivokwanilisika kuli Mulungu." ²⁸ Petulo anakamba kuti, "Ehe, tasiya vintu vonse vatu naku kukonkani." ²⁹ Yesu anabauza kuti, "Zoona, niku uzani kuti kulibe muntu wamene anasiya nyumba, kapene mukazi, kapena babale, kapena makolo, kapena bana, chifukwa cha ufumu wa Mulungu, ³⁰ wamene sazalandila vochilamo muziko ino, na muziko yamene izabwela, moyo wamene siusila." ³¹ Pamene anaitana pamozi kumi na babili kuli eve, anabauza kuti, "Onani, tiyenda ku Yelusalemu, na vintu vonse vamene vinalembewa na baneneli pali Mwana wa Muntu vizachitika. ³² Chifukwa azapelekewa kuli bantu bakunja, azanyozewa, naku muchitila va manyazi, kumutunyila mate. ³³ Bakasiliza kumumenya, bazakamupaya, koma pa siku ya chitatu azaka uka futi." ³⁴ Koma sibanamvesese chili chonse pali ivi, na mau aya yana bisiwa kuli beve, sibana mvesese vintu vamene vinakambiwa. ³⁵ Chinabwela chachitika kuti, pamene Yesu anali pafupi na Yeliko, muntu umozi wamene anali ni mpofu analki nkale mumbali mwa museu kupempa, pamene ³⁶ anamvela gulu yabantu ipita, anafunsa chamene chinali kuchitika. ³⁷ Banamu uza kuti Yesu waku Nazaleti anali kupita. ³⁸ Pamene apo ija mpofu inapunda, kukamba kuti, "Yesu, Mwana wa Davide, nichitile chifundo ine." ³⁹ Baja bamene banali kuyenda pasogolo banamukalipila uja mpofu, kumu uza kuti ankale osapanga chongo. Koma anapunda maningi, "Mwana wa Davide, nichitile chifundo ine." ⁴⁰ Yesu anaimilila naku kamba kuti uja mwamuna wamulete kuli eve. Manje pamene uja mpofu anafika pafupi, Yesu anamufunsa kuti, ⁴¹ "Nanga nichani chamene iwe ufuna kuti nikuchitile?" Anayanka kuti, "Ambuye, Ine nifuna kuti niyambe kulanga." ⁴² Yesu anakamba kuli eve kuti, "Landila menso yako." Chikulupililo chako chakupolesa." ⁴³ Pamene apo anayamba kulangana naku mukonka, uku alemekeza Mulungu. Bantu bonse, pamene banaona ivi, banatamanda Mulungu.

Chapter 19

¹ Yesu anangena ndipo anali kuyenda mu Yeliko. ² Onani, mwenze mamuna muja oitaniwa Zakeyo. Enzeli mukulu wa opoka musonkho ndipo enzeli olemela. ³ Enzo yesa kuona kuti Yeasu niuti, koma sana kwanise kumuona mugulu, chifukwa enzeli mufupi. ⁴ Mwa ichi anatamangila pasogolo pa gulu na kuwela mtengo wa mkuyu kuti amuone, chifukwa Yesu enze pafupi nakupikta iyo njila. ⁵ Pamene Yesu anafika, anayangana mumwamba na kumu uza kuti, "Zakeyo, bwela pansi musanga, chifukwa lelo niza nklala kunyumba yako." ⁶ Ndipo anaendesa nakuseluka na kumulandila nachimwemwe. ⁷ Pamene bonse bana ona ichi, bonse bana dandaula, kukamba kuti, "Ayenda kungena kutandalila munthu wochimwa." ⁸ Zakeyo anaimilila na kubauza Ambuye, "Onani, Ambuye, nizagaba pakati katundu yanga naku pasa osauka, ndipo ngati nina nama alionse pachilichonse, nuzamu bwezela kali 4. ⁹ Yesu anamu uza kuti, "Lelo chipulumuso chabwela kuli ino nyumba, chufukwa na eve nimwana wa Abrahamu. ¹⁰ Chifukwa Mwana wa Munthu anabwela kusakila na kupulumusa banthu bosoba." ¹¹ Pamene banali kumvela ivi vinthu, ana piliza kukamba na ku kamba fanizo, chifukwa enze pafupi na Yerusalemu, ndipo bana ganiza kuti Ufumu wa Mulungu wenze pafupi na kuonekela pamene apo. ¹² Ana kamba kuti, "Mwamuna winangu olemekeseka naenda kuziko yakutali kuti azilandilile ufumu naku bwelela. ¹³ Anaitana banchito bake 10 nakuba pasa ndala 10 nakuba uza kuti, 'Chitani malinda mpaka nikabwele.' ¹⁴ "Koma nzika zake zinamuzonda na kumutumila nthumi, kumba kuti, 'Sitiza vomela uyu munthu kuti lamulila.' ¹⁵ Chinachitika pamene anabwelela, atalandila ufumu, analamulila kuti banchito bamene anapasa ndalama babwele kuli eve, kuti azibe phindu yamene bapeza pakuchita malonda. ¹⁶ Oyamba anbwela pamenso pake, kamba kuti, 'Ambuye, ndalama zanu zapangilapo zinangu zili 10.' ¹⁷ "Munthu olemekeseka anamu uza kuti, 'Wachita bwino, wanchito wabwino. Chifukwa una khulupilika natungono, uzankhala na ulamulilo pa mizinda ili 10.' ¹⁸ "Wachibili anabwela, nakukamba kuti, 'Ndalama zanu, ambuye, zapangilapo zili 5.' ¹⁹ "Olemekeseka uja anamu uza kuti, 'Uzalamulila mizinda 5.' ²⁰ "Nawinangu anbwela, nakukamba, 'Ambuye, iyi ndalama yanu, yamene nina sunga munyula, ²¹ chifukwa nina kuyopani, chifukwa ndimwe munthu ovuta. Mutenga vamene simunaikemo, na kukolola vamene simunashange.' ²² Uja munthu olemekeseka anamu uza kuti, 'Na mau yako niza kuweluzi, iwe wanchito oipa. Uziba kuti ndine munthu ovuta, wotenga vamene sininaikemo, na ku kolola vamene sinina shange. ²³ Nichi fukwa chani siuna ike ndalama zanga kosungingila ndalama, kuti nikabwela nikazitenge na phindu?' ²⁴ Uja munthu wolemekeseka ana kamba kuli bamene benzeli imilila pafupi, 'Tangani ndalama zamene alinazo, na kupasa wamene ali ndala 10.' ²⁵ "Bana kamba kuli eve kuti, 'Ambuye, alinazo kudala ndala 10.' ²⁶ "Niku uzani, kuti alionse wamene ali nacho azapasiwa, koma kuli uyo wamene alibe, natungono twamene alinato tuza tengewa. ²⁷ Koma aba badani banga, baja bamene sibana fune kuti nibalamulile, beleteni kuno nakuba paya pamenso panga.'" ²⁸ Pamene anakamba ivi vinthu, anapitiliza kuyenda, kuyenda ku Yerusalemu. ²⁹ China chitika kuti pamene anafika pafupi na Betifagi na Betani, ku lupili yoitaniwa Oliveti, anatuma buphunzila bake babili, ³⁰ kubauza kuti, "Endani mu munzi okonkhapo. Pamene mungena, muzapeza mwana wa bulu wamene kalibe ku kwelewapo. Mumasuleni na kumuleta kuli ine. ³¹ Ngati alionse akufunsani kuti, 'Nichani mu mumangusulila?' mukambe kuti, 'Ambuya amufuna.'" ³² Bamene bana tumiwa banenda na kupeza mwana wa bulu monga mwamene Yesu anaba uzila. ³³ pamene benzeli kumasula mwana wabulu, benebake bana kamba kuti, "Nichani chamene mumangusulila mwana wa bulu?" ³⁴ Bana kamba kuti, "Ambuye bamufuna." ³⁵ Bana muleta kuli Yesu, na kuponya mikanjo vao pali mwana wa bulu ndipo Yesu anankhalapo. ³⁶ Pemene enzeli kuyenda, banayanzika mikanjo yao panjila. ³⁷ Pamene enze kufika pafupi na malo yamene Lupili ya Olivesi itelemukila, gulu yonse yaophunzila inyamba kusangalala naku tamanda Mulungu mo kuwa chifukwa chazinchito zikulu zamene bana ona, ³⁸ kukamba kuti, "Yodala ni mfumu yamen ibwela muzina ya Ambuye! Mutendele kumwamba na ulemelelo mumwamba!" ³⁹ Benangu pali ba falise mugulu banamu uza kuti, "Aphunzisi, kalipilani ophunzila banu." ⁴⁰ Yesu ana yahnkha naku kamba kuti, "Niku uzani, ngati benzeli zi, miyala izayamba kupunda." ⁴¹ Pamene Yesu anafika pafupi na muzinda, ana ulilila, ⁴² kukamba kuti, "Asembe chabe mwaziba musiku yalelo, nangu imwe, vinthu vamene vikuletelani mtendele! Koma nivobisika ku menso oyanu. ⁴³ Chifukwa iza fika siku pali imwe pamene badani banu bazamanga vuku zungulilani nakuku zungulilani naku kutitikizani mbali zonse. ⁴⁴ Bazaku menyani ku kugwesalani pansi, pamozi na bana banu. Sibaza siya mwala pamwamba paunzake chufukwa simuna chizindikila pemene Mulungu enzeli kuyesa ku kupulumusani. ⁴⁵ Yesu anangena mutempele naku yamba ku pilikisa baja bemene benzeli kugulisa, ⁴⁶ kubauza kuti, "Chinalembeba, 'Nyumba yanga izankhala nyumba ya pempelo, koma mwaipanga mobisama mbava. ⁴⁷ Yesu enzeli kuphunzisa masiku yonse mutempele. Bakulu ba ansembe na balembe na basogoleli babanthu benzu funa kumupaya, ⁴⁸ koma sibenzo peza njila you chichitilamo chifukwa banthu bonse benze kumumvelela maningi.

Chapter 20

¹ Siku inangu pamene Yesu anali kupunzisa bantu mu tempele naku lalika utenga wa bwino ba kulu bansembe na bolemba banabwela kuli eve pamozi na bakulu bakulu. ² Banakamba, kumu uza kuti, "Ti uze nanga ni mpavi za ba ndani zamene usebenzesa kuchita ivi vintu, kapena nindani nindani wamene anakupasa mpavu." ³ Anayanka naku bauza kuti, "Naine nizakufunsani funso imozi, muniyanke. ⁴ Nanga ubatizo wa Yohane: Unachokela kumwamba kapena kubantu?" ⁵ Banakambisana pabeka, kukamba kuti, "Ngati takamba kuti, 'Kumwamba,' azakamba kuti, 'manje nichani imwe simunanikululupile?' ⁶ Manje ngati takamba kuti, 'Ku bantu,' bantu bonse bazati tema myala, chifukwa bakululupila kuti Yohane anali muneneli." ⁷ Banayanka kuti sibaziba kwamene unachokela. ⁸ Yesu anabauza kuti, "Naine kansi sinizaku uzani mpavu zamene ine nisebenzesa kuchita ivi." ⁹ Anabauza bantu fanizo iyi, "Muntu anashanga munda wa mpesa, naku ibwelekesa kuli boshanga mpesa, naku yenda ku ziko ina kukankala ntawi itali. ¹⁰ Pa ntawi yake anatuma wantchito wake kuli balimi ba mpesa, kuti bamupaseko vipaso vamu munda. Koma baja balimi ba mpesa banamu menya, naku mubweza alibe kalikonse. ¹¹ Anabwela atuma wantchito winangu na eve banamu menya, kumuchitisa manyazi, naku mubweza alibe kali konse. ¹² Anatumiza futi wachitatu na eve bana menya, naku mutaya panja. ¹³ Manje mwine wa munda wa mpesa anakamba kuti, 'Nanga kansi nizachita chani? Nizatuma mwana wanga okondewa. Kapena eve bazamupasa ulemu.' ¹⁴ "Koma pamene balimi ba mpesa banamuona, bana kambisana pakati pao, kukamba kuti, 'uyu ndiye oloba.' ¹⁵ Tiye timupaye, kuti cholobamo chinkale chatu." ¹⁶ Banamuchosa mu munda wa mpesa nakumupaya. Kansi mwine wa munda wa mpesa azakabachita chani baja? ¹⁷ Azakabwela nakubaononga aba balimi ba mpesa, naku pasa munda kuli benangu. "Pamene bana mvula ivi, banakamba kuti, "Chisakachitike!" ¹⁸ Koma Yesu anabalanga, nakukamba kuti, "Nanga tantaugo ya ivi vamene vinalembewa nichani: 'Mwala wamene bomanga banaukana wankala mwala wapa ngondya?' ¹⁹ Ali onse wamene agwela pa mwala uja azapwanywa, nauja wamene uzamugwela azapwanywa." ²⁰ Bolemba nabakulubakulu bansembe banayesesa kuti bamugwile pantawi yamene ija, chifukwa banaziba kuti anakamba iyi fanizo kukamba pali beve. Koma banali kuyopa bantu. ²¹ Uku bali kumuyanganisisa maningi, banatuma akazitape bamene banali kuzionesa monga banali bachilungamo, kuti bamupezele kafukwa mu mau yake, mwakuti bamupeleke kuli ba kazembe bolamulila. ²² Banamufunsa kukamba kuti, "mupunzisi, tiziba kuti imwe mukamba nakupunzisa bwino, ndipo simuma gwedezewa na pamene aimilila muntu, koma muma punzisa va zoona pali njila ya Mulungu. ²³ Nanga kansi nichintu chovomelesewa kuti ise tikazi peleka misonko kuli Kaisala, kapena iyayi?" ²⁴ Koma Yesu anaziba kuchenjela kwabo, naku kamba kuti, ²⁵ "Nilangizeni dinalisi. Nanga ichi chintuntunzi nakulemba kwamene kulipo kansi nikwandani?" Banayanka kuti, "Kaisala." ²⁶ Anabauza kuti, "Kansi pasani Kaisala vintu va Kaisala, na Mulungu vintu va Mulungu." ²⁷ Sibanakwanise kupezamo cholakwa mu vamene anakamba pamenso pa bantu, koma banankala bodabwa na yanko yake, naku nkala zii. ²⁸ Pamene benangu pali ba Saduki pamene banabwela kuli eve, bamene bamakamba kuti kuli ku ukisiwa, ²⁹ banamufunsa kuti, "Apunzisi, Mose anatilembela ise kukamba kuti ngati mubale wa mubale amwalila, ngati anali na mukazi, koma analibe mwana, mubale afunika kumutenga mukazi wa mubale wake, naku nkala naye na mwana wa mubale wake. ³⁰ Panali babale ba sanu na babili umozi anakwatila, nakumwalila alibe mwana, ³¹ na wachibili na eve. ³² Wachitatu anamungena chokolo na eve, mpaka kufika wa chisanu na tubili na eve sanankale naye na mwana, nakumwalila. ³³ Kuchoka apa na mukazi uja anamwalila. ³⁴ Muku ukisiwa manje, azakankala mukazi wa uti mwamuna? Chifukwa bonse basanu na babili anankalapo mukazi wabo." ³⁵ Yesu anabauza kuti, "Bana ba muziko muno bamakwatila naku kwatiliwa. ³⁶ Koma baja bamene bamaonesewa kuti niboyenela kulandila ku ukisiwa kuchoka ku bakufa sibazaka kwatila kapena kupelekewa ku chikwati, ³⁷ Kapena kufa sibazakafa futi, chifukwa balingana na bangelo na bana ba Mulungu, kunkala bana ba ku ukisiwa. ³⁸ Koma kuti bakufa bama ukisiwa, na Mose analangiza, mumalo yamu sanga, mwamene aitana Ambuye Mulungu wa Abrahamu na Mulungu wa Isaki na Mulungu wa Yakobo. ³⁹ Manje eve si Mulungu wa bakufa, koma wa bamoyo, chifukwa kuli eve bonse bali na moyo." ⁴⁰ Benangu ba Falisi banamuyanka kuti, "Apunzisi, mwayanka bwino." ⁴¹ Chifukwa sibanafune kumufunsa mafunso yali yonse. ⁴² Yesu anabauza kuti, "Nanga nichani chamene bakambila kuti Kristu ni mwana wa Davide? ⁴³ Chifukwa Davide amakamba mu buku ya Nyimbo kuti, Ambuye banauza Ambuye banga kuti, 'Nkalani ku kwanja ya manja, ⁴⁴ mpaka pamene nizapangila badani bako kunkala mupando wa mendo.' ⁴⁵ Davide eve aitana Kristu kuti 'Ambuy, manje kansi ankala bwanji mwana wa Davide?' ⁴⁶ Mukumvela kwa bantu bonse anauza bopunzila bake kuti, ⁴⁷ "Nkalani bochenjela na bolemba, bamene bamafunisisa kuyenda mu mikanjo itali nakukonda kubapasa moni wapa dela mumalo yamalonda na ponkala polemekezewa mu sinagogo na malo yapa mwamba pa pwando. ⁴⁸ Bamadya naku manyumba ya bofelewa, nakuti baonekele bapempela ma pempelo yatali. Bantu bamu tundu uyu bazankala na chiweluzo chikulu."

Chapter 21

¹ Yesu anayangana kumwamba nakuona bantu bolemela bamene benzokufaka mosungila ndalama. ² Anaona wina muzimai ofelewa naku sauka afaka makoyini. ³ Anakamba kuti, "Niku uzeni vazo'ona uyu mukazi osauka wamasiye ayikamo zambibili kusiya na aba bonse. ⁴ Aba bonse bapeleka mpaso kuchosa vambili. Kom mukazi wamasiye, kuvutika kwake, afakamo vonse vamene anali navo." ⁵ Pamene bena banali kukamaba za tempele, mwamene anayikonzela na myala ya bwino na vopeleka, Anakamba kuti, ⁶ "Pa vintu ivi vamene mwaona, masiku yazafika pamene sipazankala mwala umozi pa muzake wamene suza pwanyika." ⁷ Chakuti banamu funsa, kukamba kuti, "Opunzisa, niliti viza chitika ivi? Nichani chiza kankala cho-onela kuti ivi vintu vizakachitika?" ⁸ Yesu anayanka kuti, "Onani kuti simunamiwa. Pakuti bambili bazaka bwela muzina yanga, kukamba kuti, 'Ndine wamene,' na, 'ntawi ili pafupi, 'musaba konke. ⁹ Muka mvela nkondo na musokonezo, musayope, chifukwa ivi vintu vizafunika kuchitika, koma chimalizilo sichiza chitika pamene apo." ¹⁰ Pamene apo enve anakamba kuli benve, ziko iza okila ziko inzake, na ufumu wuza wukila ufumu. ¹¹ Kuzankala chigumula chachikulu, ndipo njala ikulu na vilango. kuzankala vochitika voyofya na vizindikilo vikulu vochokela ku mwamba. ¹² Koma pambuyo pa ivi vintu, bazakugwilani na kumizunzani imwe, naku mupelekani ku sinagogo na mudende, kumubwelesani kuma mfumu nama kazembe chifukwa cha zina yanga. ¹³ Iza kupelekani ku ndanga ya umboni yanu. ¹⁴ Mwayicho simikizani mumitima yanu kuti musakonzেকে kuzichingilza pamene ntawi ikalibe kukwana, ¹⁵ niza kupasani mawu na nzelu kuti badani banu bonse sibazakana kapena kushushana. ¹⁶ Koma muzapelekewa ku makolo, babale, bachibululu, na banzanu, ndipo bana ba imwe muzapayiwa. ¹⁷ Bonse bazaku zondani, ndipo bena imwe muzapaiwa. Bonse bazaku zondani chifukwa cha zina yanga. ¹⁸ Olo sis imozi yaku mutu kwako sizaka onogeka. ¹⁹ Mukupilila kwanu muzapeza umoyo wanu. ²⁰ Mukaona Yelusalemu yozungulikiwa na magulu ya nkondo, zibani kuti ku wonongwewa kwake kuli pafupi. ²¹ Lekani abo bali ku Yudea batamangile lu mapili, abo bali mu muzinda ba chokemo, nabali kunja ya ziko sibafunika kungena mu muzinda. ²² Chifukwa masiku aya niyo bwezela chilengo, kuti zonse zolembewa zikakwanilisiwe. ²³ Soka kuli baza kankala nama mimba na kuli bamene bonyonsha muma siku yaja! oakati pazankala chisuso chachikulu paziko, na ukwiyo pa bantu aba. ²⁴ Baza payiwa na lupanga, na kutengewa ukapolo mumayiko yonse, na Yelusalemu azadyakiwa naba mitundu paka ntawi ya mitundu ikakwane. ²⁵ Kuzankala vo-onekelako muzuba, mu mwenze, namu ntanda, ndipo napa ziko ya pansi. Maziko yaza nkala yosakazikika, yazankala yotilima chifukwa cha ku uluma wa njanja na chi mpepo chikulu. ²⁶ Kuzankala bamuna bena bazasila mpamvu kuchokela ku manta na kuyembekezele pa vintu vamene vili ku wela pa ziko ya pansi. Mpamvu zaku mwamba zizagwedezeka. ²⁷ Pamene apo baza ona Mwana wa Muntu abwela mu mitambo na mpamvu na ulemelelo ukulu. ²⁸ Koma pamene vintu ivi vizayamba kuchitika imila itu zanu, chifukwa chiwombolo chanu chili pafupi." ²⁹ Yesu anabauza fanizo, "Langanani mutengo wamukuyu, na mitengo zonse. ³⁰ Pamene vimankala nama luba, mumaona paimwe mweka kuti ntawi ya kupya yafika. ³¹ Chimozi mozi, mukaona ivi vintu vichitika, muzibe kuti ufumu wa Mulungu ulu pafupi. ³² Zoonu niku uzani kuti, uyu mubadwe siuzaka sila mpaka ivi vintu vonse vikachitike. ³³ Kumwamba na pansi kuzakapita, koma mau yanga siyazakapita. ³⁴ "Koma zisamalileni paimwe mweka, kuti mitima zanu isazule na kumwa kochila malile na moba na voganizila va umoyo, na ija siku isaka kuvalileni mwa zizizi monga chogwilila. ³⁵ Chifukwa chizakafikila pali ali onse wamene ali namoyo mu ziko yonse. ³⁶ Koma nkalani ochenjela ntawi yonse, kupempela kuti mukankale bolimba kukwanisa kutaba vintu vonse vamene vizaka chitika, naku imilila pa menso pa Mwana wa Muntu." ³⁷ Muzuba anali kupunzisa mu tempele, usiku anali kuyenda naku kankala pa pili ya Oliva. ³⁸ Bantu bonse banabwela kuseni seni kuti bamumvele mu tempele.

Chapter 22

¹ Mnanje phwando ya buledi ilibe chofufumisa yenze kufika pafupi, yamene itaniwa Pasaka. ² Bakulu ba anseme na balembi bana kambisana mwamene banga paille Yesu, chifulkwa benzeli kuyopa banthu. ³ Ndipo Satana anangena Yuda Iscalioti, wamene enzeli umo wa bali 12. ⁴ Yuda anaenda ku bakulu banseme na baka pitao na kukamba nao mwamene angapelekele Yesu kuli beve. ⁵ Bana mvela bwino na kumvelana kuti baza mupasa ndalama. ⁶ Anavomela naku sakila danga yakuti amuchose mugulu nakumu peleka kuli beve. ⁷ Ndipo inafika siku ya buledi ulibe chofufumisa, pamene nseme ya nkhoa ya Psaka yenzufunika kupelekewa. ⁸ Ndipo Yesu anatuma Petulo na Yohane, kubauza kuti, Endani muti konzekele chakudya cha Pasaka, kuti tidye." ⁹ Bana muyankha kuti, "Nikuti kwamene mufuni kuti pangile makonzekelo?" ¹⁰ Anaba yahnka kuti, "Onani, mukangena mumzinda, munthu wamene ali na mbiya yamanzi azakumana naimwe. Mukonkheni munyumba mwamene azangena. ¹¹ Ndipo mukambe ku mukulu wanyumba kuti, "Mphunzisi akamba kuli iwe, "Chipinda cha balendo chilikuti, kwamene nizayela Pasaka na bophunzila banga?" ¹² Azakulangizani chipinda chikulu chapa mwamba chokonzewa bwino navonse. Mukonzekele vonse mwamene umo." ¹³ Ndipo bana yenda, nakupeza vonse kulingana namwamene anabauzila. Banakonzeka chakudya cha Pasaka. ¹⁴ Pamene nthawi inafika, anankhala pansi naba tumiki. ¹⁵ Ndipo nakamba kuli beve, "Nina lakalaka maningi kuti nidye iyi Pasaka pemene nikalube kunzunzuka.

¹⁶ Chifukwa nikamba kuli imwe, sinizaka idya nafuti mpaka chikafikilisiwe mu ufumu wa Mulungu. ¹⁷ Ndipo Yesu anatenga chikho, na pamene anayamika, anakamba kuti, "Tengani ichi, nakugabana pakati panu. ¹⁸ Chifukwa nikamba kuli imwe, sinizamwa futi va chipaso champesa mpaka ufumu wa Mulungu ukabwele." ¹⁹ Ndipo anatenga buledi, napamene anayamika, nau unyema, nakubapasa, kukamba kuti. "Iyi nithupi yanga, yamene ipasiwa chifukwa chaimwe. Chitani ichi mwa kunikumbukila ine." ²⁰ Anatenga chikho munjila imozi mozi pemene banasiliza chakudya chamumazulo, nakukamba kuti, "Ichi chikho ni chipangano chasopano mumagazi yanga, yamene nina kukheselani. ²¹ Koma mvesesani. Wamene azani peleka alinaine pathebo. ²² Chifukwa mwana wa munthu ayenda kulingana na mwamene chinankhazikisiwa. Koma soka kuli munthu wamene amu peleka!" ²³ Banayamba kukambisana pakati pao niuti pali beve wamene anga chite ichi. ²⁴ Ndipo panauka mukanganano pakati pao kuti nindani pali beve enzeli mkulu pabonse. ²⁵ Anakamba kuli beve kuti, "Mafumu ya bakunja ni mabwana pali beve, na bamene bali na ulamulilo pali beve baonewa monga ndiye bachita vabwino kubanhu bao. ²⁶ Koma simwamene chifunika kunkhalila naimwe, lekani wamene nimukulu maningi pakati panu ankhale monga nimungono pabonse, na wamene ali olemkezeke maningi monga wanchito. ²⁷ Chifukwa niuti mukulu maningi, wamene ankhala pathebo, nangu wamene asenbenza? Kansi siuja wamene ankhala pathebo? Koma nili pakati panu monga wanchito. ²⁸ Koma ndimwe bamene muna pitiliza naine muma yeso yanga. ²⁹ Nikupasani ufumu, na mwamene ba Tate bana nipasila ufumu, ³⁰ kuti mudye na kumwa pa thebo yanga mu ufumu wanga, ndipo muzankhala pamipando yachifumu kuweluzwa mitundu 12 ya Israeli. ³¹ "Simoni, Simoni, nkhal ochenjela, Satana afuna kukutenga, kuti akusefe monga tiligu. ³² Koma nakupemphelela, kuti chikhulupililo chako chisakangiwe. Ukabwelela futi, ulimbise babale bako." ³³ Petulo anamuyankha kuti, "Ambuye, ndine okonzeka kuyenda naimwe kundende na kuimfa." ³⁴ Yesu anayankha, "Niku uza, Petulo, tambala sazaliza siku yalelo, ukalibe kunikana katatu kuti uniziba ine." ³⁵ Ndipo Yesu anaba uza kuti, "Pamene ninakutumani na chikwama, chola chavofunikila, nagu nsapato, munasobekela chilichonse? Banyankha, "Palibe." ³⁶ Ndipo anaba uza kuti, "Koma manje, wamene ali nachikwam, lekani atenge, nachola chavofunikila. Wamene alibe lupanga agulise chovala chake nakugula imozi. ³⁷ Chifukwa nikamba kuli imwe, chamene china lembewa pali ine chifunika kufikiliziwa, 'Anapendewa pamozi na bochimwa.' Chifukwa vemene vina lodelewa pali ine vifikilisiwa." ³⁸ Ndipo bana kamba kuti, "Ambuye, onani! Malupanga yabili aya." Anaba uza kuti, "Niyo kwanila." ³⁹ Yesu anaenda, mwamen enzeli kuchitila kambuli, ku Lupili ya Oliveti, na bophunzila bana mukonkha. ⁴⁰ Pamene banafika, anakamba kuli beve, "Pempheleli kuti musangene muma yeselo." ⁴¹ Anaenda kuchoka kuli beve kamtunda kangono, ndipo anagwada naku pemphela, ⁴² kukamba kuti, "Atate, ngati mufuna, chosani ichi chikho pali ine. Koma osati chifunilo changa, koma chanu chichitike." ⁴³ Ndipo mungelo kuchokela kumwamba anaonekela kuli eve, kumu limbikisa. ⁴⁴ Mu ukali, anapemphela namutima onse, na chibe chake china sanduko monga kuthonya kwa magari kugwala pansi. ⁴⁵ Pamene ananyamuka kuchoka mupephelo, anabwela kubophunzila na kuba peza gone chifukwa cha chisoni chao ⁴⁶ na kubafunsa kuti, "Nichifukwa chani mugonela? Nyamukani nakupemphela, kuti musangene mumaeselo." ⁴⁷ Akali kukamba, onani, gulu inaonekela, na Yudas, umozi wa bali 12, enzo basogolela. Anabwela pafupi na Yesu kuti amu pyompyone, ⁴⁸ koma Yesu anakamba kuli eve kuti, "Yudas, upeleka Mwana wa Munthu na kupyompyona?" ⁴⁹ Pamene baja bamene bana zungulula Yesu bana ona vemene venzeli kuchitika, banakamba kuti, "Ambuye, timenye na lupanga?" ⁵⁰ Ndipo umozi anamenya wanchito wa mukulu wa

ansembe, nakumujuba kwatu yaku kwanja ya manja.⁵¹ Yesu anakamba kuti, "Lekani!" Anagwila kwatu yake, na kumupolesa.⁵² Yasu anakamba ku bakulu bansembe, kuli ba kapitao ba mu tempele, na bakulu bakulu bamene banabwela kumugwila, "Kansi mwabwela kugwila mbava, nama lupanga na vomenyela?"⁵³ Pamene ninali naimwe masiku yonse mutempele, simuna ike manja yanu pali ine. Koma ino nithawi yanu, na ulamulilo wamdima."⁵⁴ Kumugwila, banamu peleka naku mu bwelesa munyumba ya mukulu wa ansembe. Koma Petulo naba konkha pambuyo kamtunda pangono.⁵⁵ Pambuyo pa yasha mulilo pakati kabwalo na kunkhala pansi, Petulo anankhala pakati kao.⁵⁶ Wanchito winagu mukazi anamuona ali nkhole mukusanika kwamulilo, na kumu yanganisisa nakukamaba kuti, "Uyu munthu enzeli naye."⁵⁷ Koma Petulo anakana, kukamba kuti, "Muzimai, ine sinimuziba."⁵⁸ Pamene pana panapita kantawi kangono nawinangu anamuona, nakukamba kuti, "Naiwe ndiwe umozi mwa beve." Koma Petulo anakamba kuti, "Iwe munthu, sindine."⁵⁹ Pamene panapita ola imozi munthu winangu analimbikila na kukamba kuti, "Zoona uyu munthu naeve enzeli nae, chifukwa ni waku Galilea."⁶⁰ Koma Petulo anakamba kuti, "Iwe munthu, ine siniziba vamene ukamba." Pamene apo, akali kukamba, tambala analila.⁶¹ Kupindamuka, Abuye bana yangana Petulo, na Petulo anakumbukila mau ya Ambuye, pamene bana kamba kuli eve kuti "Pamene tambala akalibe kulila lelo uzani kana katatu."⁶² Petulo enaenda panja nakulila naukali.⁶³ Ndipo bomulonda Yesu bana munyoza nakumu menya.⁶⁴ Banamu vinikila, nakumu funsa, kukamba kuti, "Nenela! Nindani wamene akumenya?"⁶⁵ Banakamba vambili kumunamizila Yesu, kumunyoza Yesu.⁶⁶ Pamene kunacha chabe, bakulu bakulu ba banthu bana kumana pamozi, bonse na bakulu bansembe na balimbi. Bana mupeleka kubwalo yao⁶⁷ nakukamba kuti, "Ngati ndiwe Kristu, tiuze." Koma anaba yankha kuti, "Ngati naku uzani, simuzani khulupilila,"⁶⁸ ndipo ngati nakufunsani sumuzayankha.⁶⁹ Koma kuyamba manje na kuyenda kusongolo, Mwana wa Munthu azankhala ku kwanja yamanja ya mphamvu za Mulungu."⁷⁰ Bonse banakamba kuti, diye kuti ndimwe Mana wa Mulungu?" Yesu anabauza kuti, "Ndimwe mukamba kuti ndine."⁷¹ Ndipo bana kamba kuti, "Nichifukwa chani tikali kufunila mboni? Chifukwe ise tazimvelela ku chika pakamwa pake."

Chapter 23

¹ Gulu yabo yonse insnyamuks nakuleta Yesu kuli Pilato. ² Anayamba kumupasa milandu, nakukamba kuti, "tamuoze muntu uyu osobesa ziko yabantu, kubalesa kupasa musonko kasala, kuti enve ni Kristu, Mfumu." ³ Pilato anafumufunsa, nakamba, "Ndiwe mfumu ya Yuda?" Yesu anamuyanka akukamba "iwe wakamba." ⁴ Pilato anakamba kuli bakuli bansembe kumagulu, "Sininapezamo mulandu muli uyu muntu." ⁵ Koma bana limbikila, nakukamba, "asokoneza bantu, kupunzisa mu Yudeya yonse kuyambia ku Galileya mpaka kufika kumalo kuno." ⁶ Pamene Pilato ananvela ivi, anafunsa kapena uyu muntu niku galileya. ⁷ Pamene anaziba kuti alimu mulamulilo wa Herodi, anamutumiza Yesu kuli Herodi, naenve anali ku Yelusalemu pamasiku yaja. ⁸ Pamene herodi anaona Yesu, anakondwela maningi, chifukwa analikana kumuona. anavela pa eve anaukufuna kuona wodabwisa vamene anali chita. ⁹ Herodi anafunsa Yesu namau yambili, koma Yesu sanamuyanka chili chonse. ¹⁰ Bakulu ba bansembe na bolemba anaimilila, nakumupasa milandu. ¹¹ Helodi nabasilikali bake namumunyoza Yesu banatukana naku nakumunyoza. namanukila nakuvalika vovala va chifumu nakumubweza kuli Pilato. ¹² Pakuti Helodi na Pilato banayamba kunverana kuyambambila pasika yamene ija, vikalibe kuchika ivi, sinali sibanali kunvelana. ¹³ Pamene apo Pilato anaitana bakulu bansembe pamozi bolamulila na gulu ya bantu ¹⁴ anakamba mwanileta uyu muntu monga wamene asobesa bantu ndipo onani, ine, namufunsa pamenso fanu. sinapeze mulundu muli uyu muuynu kulingana ivo vintu vame munane zila. ¹⁵ Kulibe, kapena olo Helodi, chifukwa amubweza kuli ise, loma onani, kulibe chamene achita kuti apayiwe. ¹⁶ Nizamupa chilango nakukulekelela." ¹⁷ **Mapepela yakudala yambili yalibe Luke 23:17, anamu funikila kumasula umozi wa mangiwa pabomangiwa ila pwando la a..... ¹⁸ Koma bapunda pamozi, nakuma "muchoseni apa uyu muntu, Tichoseleni Banabasi! ¹⁹ Balaba anali muntu wamene anafakiwa mundende chifukwa cha musokonezo mumuzinda napaya nakupaya muntu. ²⁰ Pilato anakamba nabo futi, kufunisisa kuti bamusiye Yesu. ²¹ Koma banapunda, kukamba kuti, "Mupachikeni, mupachikeni." ²² Anabauza kachitatu futi kuti, "Chifukwa chani, nichoipa bwanji chamene achita uyu muntu kansi? Ine sininapezemo chilichonse chamene chiyenela kumupaya. Nikamulanga, nizamula." ²³ Koma banali bolimbikila na liu yokwela pamwamba, kufunisisa kuti eve apachikiwe. Mau yawo yanamveka kuli Pilato. ²⁴ Pilato anasanka kubapasa vamene banali kufuna. ²⁵ Anamasula wamene beve banali kufuna wamene anali mundende chifukwa cha ku chipongoo na kupaya. Koma ana peleka Yesu monga mwamene banali kufunila. ²⁶ Pamene banali kuyenda naye, banagwila umozi muntu zina yake Simoni waku Sailene, wamene anali kuchokela ku munzi, banaika mutanda pali eve kuti aunyamule, kukonka Yesu. ²⁷ Gulu ya bantu ikulu, ya bakazi bamene banali bovutika mitima nakumulila, banali kumukonka pambuyo. ²⁸ Koma pamene anapindamukila kumbuyo, Yesu anabauza kuti, "Bazimai bamu Yelusalemu, musanililile ine, koma zililileni mweka na bana banu. ²⁹ Chifukwa onani manje, masiku yazabwela yamene bazakamba kuti, 'Bodalisika nibaja bamene bakangiwa kubala na mimba zamene sizina balepo, na mabele yamene siyananyonshepo.' ³⁰ Pamene apo bazayamba ku uzala malupili kuti, 'Tigwele iwe,' na ku tuma chulu kuti, 'Tibise iwe.' ³¹ Chifukwa ngati bakamba ivi vintu pamene mutengo ukalibe kuyuma, nanga nichani chamene chizachitika pamene uzakayuma?" ³² Bamuna benangu, bachifwamba babili, banaba tengela pamozi na eve kuti aikiwe ku imfa. ³³ Pamene banabwela kumalo yoitaniwa kuti "Bade," kwamene kuja banamupachika pamozi na vigabenga-umozi ku kwanja ya manja wina ku kwanja ya manzele. ³⁴ Yesu anakamba kuti, "Atate, bakululukileni, chifukwa sibaziba chamene bachita." Pamene apo bana teya njuga, kugabana vovala vake. ³⁵ Bantu banaimilila kutamba pamene basogoleli banali kumu nyoza, kukamba kuti, "Anapulumusa benngu. Mulekeni zipulumuse, ngati ni Kristu wochokela kuli Mulungu, wamene anasankiwa." ³⁶ Basilikali na beve banamuzyoza, kufika pafupi na eve, kumupasa vinyu, ³⁷ nakukamba kuti, "Ngati ndiwe Mfumu wa ba Yuda, zipulumuse weka." ³⁸ Panali futi na chikwangwana pamwamba pake, "Uyu ndiye Mfumu wa ba Yuda." ³⁹ Umozi pali vigabenga vija anamu nyoza kumu uza kuti, "Nanga iwe sindiwe Kristu? Zipulumuse weka pamozi na ise." ⁴⁰ Koma winangu anamukalipila, kukamba kuti, "Nanga iwe siuyopa Mulungu, chifukwa tili na chilango chimozi?" ⁴¹ Ise ni zoona tili pano chifukwa tiyenela, tilandila vamene viti linga chifukwa cha vamene tinachita. Koma uyu muntu kulibe cholakwa chamene anachita. ⁴² Ndipo anakamba kuti, "Yesu, ukanikumbukile pamene uzangena mu ufumu wako." ⁴³ Yesu anamu yanka kuti, "Zoona niku uza iwe, lelo uzankala pamozi naine mu paladizo." ⁴⁴ Inali ntawi ya 12 koloko ya muzuba, mudima unabwela pa ziko yonse kufikila ntawi ya 15 koloko ⁴⁵ ntawi yamene zuba si ina onekele. Pamene apo chisalu cha mu tempele china ng'ambika pa bili. ⁴⁶ Kulila na liu yapamwamba, Yesu anakamba kuti, "Atate, naika mumanja yanu muzimu wanga." Pamene anakamba ivi, anamwalila. ⁴⁷ Pamene mukulu wa asilikali anaona vamene vinachitika, analemekeza Mulungu, kukamba kuti, "Ni zoona uyu muntu anali olungama." ⁴⁸ Pamene magulu yonse yanabwela pamozi kuona ivi vintu yanaona vamene vinachitika, banabwelela uku bazimenya pa chifuba beka. ⁴⁹ Koma bonse baja bamene banali kumuziba, na bazimai bamene banali kumukonka pambuyo kuchokela ku

Galileya, banaimilila patali, kutamba ivi vintu.⁵⁰ Ndipo onani, panali muntu zina yake Yosefe, wamene anali mukulu wa milandu. Eve anali muntu wabwino nafuti wachilungamo.⁵¹ Uyu muntu eve sanali ana vomelezana nabo ba milandu pa chiweluzo chabo na vamene banachita. Anali ochokela ku muzinda wa Aimatiya waku Yudeya, anali kusakila ufumu wa Mulungu.⁵² Uyu muntu, pamene anafika kuli Pilato, anapempa thupi ya Yesu.⁵³ Anatenga mutembo, nakuivalika mu nsalu yopepuka, naku uika mumanda yamene yanapangiwa ku mwala, mwamene sibenze bana ikamo muntu ali onse kumbuyo.

⁵⁴ Inali siku yokonzeka, na Sabata inali pafupi kuyamba.⁵⁵ Bazimai bamene banabwela na Yesu kuchokela ku Galileya nakuona mwamene tupi yake inaikiliwa.⁵⁶ Banabwelela naku konza vonunkila na mafuta. Pa Sabata bana pumula kulingana na lamulo.

Chapter 24

¹ Kuseni-seni pa siku yoyamba ya sabata, banabwela kumanda, kuleta vonunkila vamene banakonzekela. ² Banapeza chimwala chinachosewapo pa manda. ³ Pamene banangena mukati, koma sibanapeze mutembo wa Ambuye Yesu. ⁴ Chinabwela chachitika futi kuti, pamene bakanali bosokonezeka pali ichi, mwazizizi, bamuna babili banaimilila pafupi na beve mu mikanjo zobeka. ⁵ Pamene bakazi baja banali bozula na manta nakugwa pamenso pawo, banakamba kuli bazimai kuti, "Nanga kansi nichani musakila bamoyo pa bakufa?" ⁶ salipano, koma aukisiwa! kumbukilani mwamene anakambisilani pamene anali akali mu Galile, ⁷ kukamba kuti mwana wa muntu azapasiwa mumanja yabantu bochimwa naku pachikiwa, ndipo azukisiwa pasiku yachitatu." ⁸ Bazimai banakumbukila mau yake ⁹ naku bwelela kuchokela ku manda nakuuza ivi vintu vonse kuli bali 11 na bonse. ¹⁰ manje Maria Magadlena, Joana, Maria amai bake Yakobo, naba bazimai benangu bemene banali nabo banauba ivi vintu kuli ba tumiki. ¹¹ koma utenga uyu unaoneka monga niku kukamba kwachabe chabe kuli ba tumiki, ndipo sibana mukulupile muzimai. ¹² koma Petulo ananyamuka naku tamangila ku manda, na, kubelama nakulanganamo, anaona nyula zopepuka zili pazeka. kuchokela apo Petulo anayenda kunyumba yake, odabwa kuti nichani chamene china chitika. ¹³ Onani, babili pali beve banali kuyenda yamene ija siku ku munzi wa Emawusi, wamene unali muzinda wofikila ma kilomita 10 kuchokela ku Yelusalemu. ¹⁴ Banakambisana pa beka pali vintu vamene vinachitika. ¹⁵ Chinachitika kuti, pamene banali kukambisana naku zifunsa ma funso beka, Yesu mwine wake anafika pafupi na beve nakuyenda nabo pamozi. ¹⁶ Koma menso menso yabo siyanali yoseguka kuti bamuzibe. ¹⁷ Yesu anabauza kuti, "Kansi nichani kamene imwe babili mukambapo pamene muyenda?" Banaimilila bomvesana nachifundo. ¹⁸ Umozi pali beve, zina yake, Kleyopas, anamuyanka kuti, "Kansi nanga ndiwe weka mu Yelusalemu wamene saziba vintu vamene vinachitika aya masiku?" ¹⁹ Yesu anabauza kuti, "Niviti vintu kansi?" Banamuyanka kuti, "Vintu vamene vikamba pali Yesu waku Nazaleti, wamene anali muneneli, wampavu muvochita namu mau pamenso pa Mulungu na bantu bonse, ²⁰ na mwamene bakulu bakulu ba nsembe na basogoleli batu banamupeleka kuti aweluziwe chiweluzo cha imfa nakuti apachikiwe. ²¹ Koma ise tinali nachiyembekezo kuti eve ndiye wamene azapulumusisa Izilayeli. Zooni, nakuchilapo apa, iyi ni siku ya chitatu kuchokela pamene ivi vintu vinachitika. ²² Koma nafuti, bena bakazi pagulu yatu banatidabwisa, banali kumanda kuseni seni. ²³ Pamene beve sibana ipeze tupi yake, banabwela, banali kukamba kuti banaona manso mpenya yaba ngelo bamene bana kamba kuti ali na moyo. ²⁴ Benangu bazi bambo bamene banali pamozi naise bana enda kumanda, nakupeza monga mwamene bazimai banakambila. Koma sibanamuone." ²⁵ Yesu anabauza kuti, "Imwe bamuna bopusa wochedwa kumutima kuti bakululupilile mu vonse vamene baneneli banakamba! ²⁶ Kansi sichintu chamene chinali chofunikila kuti Klistu ayenela kuvutika vintu ivi, naku ngena mu ulemelelo wake?" ²⁷ Chokonkapo kuyambila pali Mose kufikila mpaka ba neneli bonse, Yesu anabamasulila vintu vamene vinali kumukuza mu malemba yonse. ²⁸ Pamene banayamba kufika pafupi na kumunzi kwamene banali kuyenda, Yesu anachita monga anali kupitilila. ²⁹ Koma banamu kakamiza, kumu uza kuti, "Nkalani naise, chifukwa ni ntawi yaku mazulo ino kazuba kwasala pang'nono kuti kangena." Pamene apo Yesu ana enda kukankala nabo. ³⁰ Chinachitika mwakuti, pamene eve anankala panso nabo kuti adye, anatenga buledi, anaidalisa, nakuigaba, nakubapasa. ³¹ Pamene apo menso yabo yana seguka, nakumuziba, anasoba naku soba kuchoka pamenso yabo. ³² Banakambisana beka kuti, "Nanga mitima zatu sizenze kupya mukati mwati, pamene eve anali kutikambisa munjila, pamene anali kuti uza malemba ise?" ³³ Banaima ntawi yamene iyo naku bwelela ku Yelusalemu. Banapeza batumiki kumi na umozi banabwela pamozi nabaja bamene banali nabo, ³⁴ bakamba kuti, "Ambuye ba ukisiwa zooni, bana onekela kuli Simoni." ³⁵ Banashimika vintu vamene vinabachitikila munjila, na mwamene Yesu anaonekela kuli beve pogaba buledi. ³⁶ Pamene banakamba ivi vintu, Yesu anaimilila pakati pabo, naku bauza kuti, "Mutendere kuli imwe." ³⁷ Koma banali banayopa nakunkala bozula na manta, nakuyamba kuganzila kuti kapena baona chibanda. ³⁸ Yesu anabauza kuti, "Nanga nichani kansi muvutika mutima? Kansi nichani muli namafunso mumitima zanu?" ³⁹ Onani manja yanga na mendo yanga, kuti ndine. Nigwileni kuti muone. Chifukwa muzimu ulibe nyama kapena mafupa, monga mwamene ine nilili nayo." ⁴⁰ Pamene anasiliza kukamba ivi vintu, anabalangiza manja yake na mendo yake. ⁴¹ Banakangiwa kukululupilila chifukwa cha chimwemwe, ndipo bana dabwa. Yesu anabauza kuti, "Muli na vakudya vili vonse?" ⁴² Banamusunila nsomba yoshoka nakumupasa, ⁴³ anaitenga nakudya mumenso mwabo. ⁴⁴ Anabauza kuti, "Pamene ine ninali naimwe, ninaku uzani vonse vamene vinalembewa mumalamulo ya Mose na baneneli na Manyimbo kuti viyenela kukwanilisika." ⁴⁵ Pamene apo anabasegula nzeli zabo, kuti bazibe malemba. ⁴⁶ Anabauza kuti, "Mwamene umu ndiye mwamene chinalembewa, kuti Klistu ayenela kuvutika naku uka futi kubakufa pa siku ya chitatu. ⁴⁷ Kutembenuka naku kululukiliwa kwa machimo kuyenela kulalikiliwa mu zina yake mu maiko yonse, kuyambila mu Yelusalemu. ⁴⁸ ⁴⁹ Imwe ndimwe mboni za ivi vintu. Onani, ine nikutumilani chamene ba

Tate banalonjeza. Koma yembekezani mu muzinda mpaka mukavalikiwe na mpavu zochokela kumwamba."⁵⁰ Pamene apo Yesu anaba sogolela mpaka kuyena kukafika pafupi na Betani. Anaimya manja yake naku badalisa.⁵¹ Chinachitika kuti, pamene anali kubadalisa, anabasiya anatengewa kuyenda kumwamba.⁵² Pamene apo banamu pembezanaku bwelela ku Yelusalemu na chimwemwe chikulu.⁵³ Banali kupezeka mu tempele ntawi yonse, kulemekeza Mulungu.

John

Chapter 1

¹ Pachiyambi panali mau ,ndipo mau anali ndi Mulungu,ndipo mau anali Mulungu. ² uyu anali pachiyambi ndi Mulungu. ³ Zonse zinalengedwa na iye ndipo palibe chamene chinalengedwa popanda iye. ⁴ Mwayeve mwenze umoyo na umoyo wenzeli kuunika kwabanthu onse. ⁵ kuunika kunaonekela mumdima koma mudima siunakwanise kuigonjesa. ⁶ Penze munthu wamene anachokela kwa Mulungu amene anali Yohane ⁷ Anabwela kupeleka umboni nyali kuti anthu onse akakhulupilile kupitila mulieve. , ⁸ Yohane sanali Nyali koma anabwela kupeleka umboni kuti nyali. ⁹ Inali nyali yazoona isanika ku anthu onse lapansi,yamene inabwela mu ziko lapansi. ¹⁰ Eve enze muziko lapansi na vonse ¹¹ Niyeve anavipanga koma sibanamuzibe,anabwela kubanthu bake koma sibanamulandile nafuti sibanamukhulukile ¹² koma kuli onse anamulandila,anamukhulupilila anabapasa mupata kunkhala bana ba Mulungu. ¹³ osati bana obadwa na mwazi kapena kubadwa muchifunilo cha munth, koma obadwa mwachifunilo cha Mulungu. ¹⁴ Mau anasanduka munthu nabwela kunkhala pakati ise ,tinaona ulemelelo wohekela kwa iye yeka ochokela kwa Atate,wozula na chisomo na choonadi. ¹⁵ Yohane anachitila umboni paliyewe ,nakupunda kuti"Uyu niwamene ninakambapo,iye obwela pasogolo,apambana ine pakuti analiko. ¹⁶ koma kuchokela kwayeve kuchokela chisomo pamwamba pa chisomo, ¹⁷ lamulo inabwela na Mose koma cisoma na choonadi vinabwela na yesu Christu. ¹⁸ kulibe wamene anaona mulungu panthawi iliyonse,.Mulungu yeve eka wamene apumulila pachifuwa cha Atate,Amene apumulila pa chifuba cha Atate ndiye avumbulusa Atate. ¹⁹ Uyu ndiye umboni wa Yohane pamene Ayuda atuma Ansembe na Alevy kuchokela ku Yerusalemu kumufunsa kuti "Nanga ndiwe ndani ?Ndiwe Eliya,ndiwe Muneneri kapena ndiwe mesiya?" ²⁰ Yohane anabauza vazooka kuti ine sindine Christu, ²¹ Anamunsa nishini ndiwe ndani?Eliya?Anakamba kuti sindine,Nanga ndiwe muneneri?anati sindine ²² Banamufunsa Yohane kuti tiuze ndiwe ndani kuti tipeleke yankho kuli bamene batituma,"ukamba chani pali wemwine?" ²³ Anabayankha kuti ine ndine chabe mau yofuula mu chipululu kuti " konzani njira yambuye siteleti,monga momwe muneneri yesaya ananenera. ²⁴ Baja bamene banatumiwa anatumiwa na Afarisi ²⁵ Amufunsa kuti "Nanga nichifukwa ninji ubatiza banthu pamene wakana kuti sindiwe Eliya,Muneneri kapena Christu?" ²⁶ Yohane anabayankha kuti Ine nibatiza na manzi,koma alipo pakati kanu wamene simuziwa,wamene nansapato zake sinikwanisa kumasula, ²⁷ Abwela pasogolo panga. ²⁸ zonsezi zinachitika ku Berthany kuja kumbali kwa Yolodani,kwamene Yohane anali kubatiza. ²⁹ Kuseni kwakaena Yohane anaona Yesu alikubwela kwa eve nokamba ati""Taonani Nkhosa yochokela kwa Mulungu amene achosa machimo laziko lapansi. ³⁰ Uyu niwamene ninakambapo kuti kuli wamene azabwela wamene,iye wamene abwela pambuyo panga "nimukulu kuchila ine chifukwa analiko, ³¹ sininamuzibe koma chinkhala tele kuti akavumbulusidwe kwa Israeli kuti ninabwela kubatiza na manzi.. ³² Ndipo Yohane anachitila umboni kuti ninaona muzimu Oyera alikubwela pa iye monga nkhunda kuchokela kumwamba,muzimu unakhala pa eve. ³³ sininamuzindikile iye koma amene ananituma kubatiza na manzi ananaiusa kuti amene Muzimu uzasikila,nakukhala paiye. ndiye wamene abatiza ndi Muzimu Oyera. ³⁴ nayangana nakuchitila umboni kuti nimwana wa Mulungu. ³⁵ Kuseni kokonkhapo Yohane anali naophunzila bake babili ³⁶ ,Anaona Yesu alikuyenda nati" Taonani Nkhosa ya Mulungu" ³⁷ Ndipo ophunzila ace anamumvela alikulankhula izi ³⁸ Ndipo anamulondola iye.ndipo yesu anabafunsa kuti "mufuna chani ,anati muphunzisi kubondi nikuti?" ³⁹ Anati Tiyeni mukaone anapita naye yesu kunyumba kwake chifukwa inalinso nthawi yamumazulo. ⁴⁰ Umozi waiwo amene anamvela Yohane kulankhula nalondola Yesu anali Andeleya mubale wa simon Petro, ⁴¹ Anapeza mubale wake Petro poyamba namuusa nati"Tamupeze Mesiya(kutanthauza Christu) ⁴² Atamubwelesa kwa Yesu anaona iye ,Anati "Ndiwe Simon mwana wa Yohane koma kuyambila lelo uzachedwa Cephas(kutanthauza Petro) ⁴³ Siku yokonkhapo pamene Yesu anafuna kupita ku Galileya akumana ndi Philip ndipo anamuusa kuti amulondole. ⁴⁴ Manje Philip anali kuchokela ku Betsaida komwe Andeleya ndi Petro anali kuchokela. ⁴⁵ Pamene philipe anapeza Natan anamuusa nati Tamupeza uja wamene Mose anakambapo mumalamulo na aneneri kale paja ,mwana wa Yosefe waku Nazareti. ⁴⁶ Natan anafunsa Philip kuti "Nichani Chabwino chingachoke ku Nazareti?Ndipo anati tiye uwone, ⁴⁷ Pamene Yesu anamuona anati "Taonani Israeli weni weni amene mwaiye mulibe chinyengo. ⁴⁸ Natan

anafunsa kodi waniziba bwani?Yesu anamuuza kuti pamene mukalibe kuwonana na Philip Nenze nakuona ninshi ulinkhale panyansi pa chimtengo cha Mkuyu.⁴⁹ Ndipo Natan anamuyankha kuti Muphuzisi ndinu mwana wa Mulungu,⁵⁰ Ndimwe mfumu ya israeli. Yesu anamuuza kuti , chifukwa chakuti nakuona panyansi wa mtengo waMkuyu ndiye pamene ukhulupilila? Yesu anamuuza kuti uzaona vikulu kupambana ivi.⁵¹ Nikamba chazooona kwaiwe uzaona kumwamba kuzaseguka nangelo ba Mulungu nakwela nakuseluka pali mwana wamunthu.

Chapter 2

¹ Panapita masiku yatatu pamene kunankhala ukwati ku kana wa ku Galileya, na amai bake ba Yesu analiko ku ukwati uyu. ² Yesu ndi opunzila bake anaitanidwa ku pezekako ku ukwati. ³ Kunapezeka kuti vinyu inasila, amai bake Yesu ana muuza kuti, "vinyu yasila." ⁴ Yesu anakamba kuti, "muzimai, nichani ubwela kuline? popeza kuti ntawi yanga ikalibe kufika." ⁵ Amai bake ba Yesu banauza banchito kuti, "chilichonse chamene akamba kuli iwe, chitani." ⁶ Panapezeka kuti, kunali nongo zili 6 zamene zinali kusebenza mumwambo wosambilamo waba yuda, iliyonse inali na muyeso wa 80 na 120 litazi. ⁷ Yesu anabauza kuti, "azuzye aya manongo na manzi". Ndipo banazulisa maningi. ⁸ Ndipo anauziwa banchito, "kutengamo manzi ena na kupasa mukulu ogabanisa." Ndipo anachita. ⁹ Uyu mukulu ogabanisa manzi pamene analabamo mu manzi, anapeza kuti ni vinyu, chinamudabwisa koma, (banchito bamene banatapa yaja manzi banali kuziba). Anaitana mukwatibwi ndipo anamuza kuti, ¹⁰ Uyu mukulu ogabisa anapita ku mukwatibwi nakumuza kuti, "Muntu aliyense apasa vinyu vabwino pachiyambi ndipo zo chipa kumasilizilo kuchila manje." ¹¹ Ichi chinali chodabwisa choyamba chamene Yesu anachita mumuzinda wa kana wa mu Galileya. Anavumbulusa ulemelele wake ndipo wopunzila bake banakulupilila. ¹² Kuchoka apo Yesu, bamai bake, babale bake, na wopunzila bake banapita ku kapenamu na kunkalako masiku yango'no. ¹³ Manje ntawi ya paskha yaba yuda inali pafupi, ndipo Yesu anayenda ku yelusalema. ¹⁴ Yesu anapeza ogulisa ng'ombe, mbelele, na nkunda nawochinjanisa ndalama balinkale. ¹⁵ Ndipo anapanga mukwapu nakuchosamo bonse mukachisi, kufakilako mbelele na ngo'mbe. Anachosa baja bamalonda wochinja ndalama na kupindimula ma tebulo yao. ¹⁶ Kuli baja wogulisa nkunda anabauza kuti, "chosani ivi vonse, Siyani kusandusa nyumba yaba tate kunkala yogulisilamo." ¹⁷ WopunzhiLa bake Banakumbuka kuti nicholembenwa, "kuti chilakolako cha nyumbayanu chanidya". ¹⁸ Pamene apo bayuda bana mufunsa kuti, "kodi ni chiziwiso chabwanji chamene muzatilangiza, chifukwa muchitilamo zonse izi". ¹⁹ Na Yesu anabauza kuti, "Pwanyani kachisi iyi, ine nizamanga masiku yatatu." ²⁰ Koma, bakulu ba yuda banakamba kuti kodi, ungamange bwanji kachisi iyi mumasiku yatatu popeza kuti tinamanga mu zaka zili 46"? ²¹ Koma, Yesu anali kukamba pakachisi yatupiyake. ²² Pamene anauka kubakufa, ophunzila bake banakumbukila chamene Yesu anakamba mumalemba mumakambidwe yake na kukulupilila malemba yamene anakamba. ²³ Koma pamene anali phwando ya pasakha muyelusalemu, bambili bamene banabwela bana kulupilila muzina yake pamene banaona zichitidwe zake. ²⁴ Koma, Yesu sianakulupilile ali onse chifukwa analikuziba zinali mumutima mwao, ²⁵ chifukwa sianalikufunikila wina kupasila umboni pa munthu chifukwa analikuziba zonse zamukati mwamunthu.

Chapter 3

¹ Koma kunali mu farisi oyitanidwa Nikodema, musogoleli wa Ayuda. ² Uyu muntu anabwela kuli Yesu usiku na kufunsa, "Apunzisi, tiziba kuti ndimwe apunzisi ochokela kwa Mulungu chifukwa kulibe wamene angachite zodabwisa ngati sachokela kwa Mulungu." ³ Yesu ana yanka ati, "chonadi, chonadi, ngati muntu sanabadwe mwasopano, sangaone ufumu wa Mulungu." ⁴ Nikodema ana kamba kuli iye, "Kodi munthu angabadwe kachibiri ngati ni mukulu?" Sangabadwe kabiri mumimba yaba maibake, kodi chingachitike?" ⁵ Yesu ana yanka, "chonadi, chonadi, ngati muntu sanabadwe ku manzi na ku mu Zimu, sangalowe mu ufumu wa Mulungu." ⁶ Obadwa ku tupi ni tupi, obadwa ku mu Zimu ni muzimu. ⁷ Usadabwe kuti na lankula kuri iwe, 'ufunika kubadwa mwasopano.' ⁸ Mpepo imachayika konse kwamene ifuna; umavela chongo, koma suziba kwe ichokela na kwamene iyenda. Niponso, ndiye onse amene anabadwa mwa mu Zimu. ⁹ Nikodema ana yanka kwa iye ati, "zingateke bwanji izi?" ¹⁰ Yesu anayanka kwa iye, "kodi ndiwe mupunzisi wa Isirayeli, ndiponso sunvesesa izi zinthu?" ¹¹ Chonadi, chonadi, ni kuuza iwe, ti lankula vetiziba, ndiponso tilina umboni pali vamene tinaona. Koma suvomela umboni watu.

¹² Ngati na kuwuzwa pa zintu za pa ziko ndiponso sunakulupirile, uzakulupirila bwanji zintu za kumwamba? ¹³ Kuribe ana pita ku Mwamba koma iye wamene ana bwela kuchokela ku Mwamba: Mwana wa Muntu. ¹⁴ Monga Mose ana kwezeka njoka m'chipululu, chimozi mozi Mwana wa Muntu ayenera kukwezedwa, ¹⁵ kuti onse akulupirila mwa iye azankhala na umoyo osata. ¹⁶ Pakuti Mulungu anakonda ziko lapansi, ndiponso anapasa mwana wake iye yekha kuti onse wakulupirila iye asatayike koma ankale na umoyo osata. ¹⁷ Pakuti Mulungu sanatume mwana wake paziko lapansi kuti akaweruze ziko lapansi koma kuti likapulumusidwe ndi iye. ¹⁸ Onse amene akulupirila mwa iye sazakeruzidwa, koma amene sakulupirila iye azaweruzidwa chifukwa sana kulupirile mu zina ya Mwana wa Mulungu yekha. ¹⁹ Koma ciweruziro ndi ici: kuti nyali ya bwela pa ziko lapansi, ndiponso anthu ana kondesesa mu dima kuchila nyali cifukwa machitidwe yao yanali yoipa. ²⁰ Pakuti onse amene akonda zoipa azonda nyali elo sanga bwele ku nyali chifukwa machitidwe yake yanga onekele. ²¹ Koma ochita chonadi abwela ku nyali kuti nchito zake, zionekere kuti zinachitidwa mwa Mulungu." ²² Ku choka apo, Yesu ndiwo punzila bake anapita kuziko la Yudeya. Kuja ana nkala na apunzisi ake na kubatiza bantu bambiri. ²³ Manje Yohane anali kubatiza mu Ainoni pafupi na Salimu chifukwa kunali manzi yambiri. Bantu banari kubwela kwa iye ndiponso anabatiziwa, ²⁴ pakuti Yohane anali akalibe kutayiwa mu jere. ²⁵ Pameneapo panauka kushushana pakati ka ena apunzisi aYohane ndi umozi wa aYuda kamba ka mwambo osambikana. ²⁶ Ba nayenda kuli Yohane nakukamba kuli iye, "Apunzisi, uja wamene mwenze naye kumbali ya musinje wa Chimana cha Yodani, apasila umboni, onani, ali kubatiza, elo bonse bamukonka iye." ²⁷ Yohane ana yanka ati, "Munthu sangalandile koma chapasidwa kuchokela ku mwamba." ²⁸ Imwe mweka mungapase umboni kuti anakamba, 'Ine sindine Christu' koma, 'Nina tumiwa pamene akalibe kubwela.' ²⁹ Mukwati nimukazi wa kwatibwi. Manje munzake wa mukwatibwi, wamene amaimilila nakumvela, amasangalala maningi chifukwa cha liwu lamukwatibwi. Nimuli ichi, mwamene chisangalalo changa chisilizika. ³⁰ Iye afunika kukula, koma ine nichepe. ³¹ Iye wochokela Kumwamba ni wopambana kuchila zonse. Iye ana chokela paziko ni wapaziko ndiponso alankhula zapaziko. Iye wamene achokela Kumwamba achila zonse. ³² Amapasa umboni pazamene awona nakumvela, koma kulibe avomeleza umboni wa iye. ³³ Iye amene ana landila umboni avomekeza kuti Mulungu ndi chonadi.

³⁴ Iye wamene Mulungu ana tuma amakamba pa mawu ya Mulungu. Samapasa muzimu ndi muyeso. ³⁵ Atate anakonda Mwana ndiponso anapasa zinthu zonse mumanja yake. ³⁶ Iye amene akhulupilira mu Mwana azankala na umoyo wosata. Koma amene savelela Mwana sazakaona umoyo, koma ukali wa Mulungu uzankala pali iye.

Chapter 4

¹ Manje pamene Yesu anaziba kuti Bafalisi bananvela kuti Yesu anali kupanga na batiza bopunzila ba mbili kuchila Yohane ² (chingankale siYesu wamene anali kubatiza koma bopunzila bake ndiye banali kubatiza), ³ Anachokamo mu Yudeya nakubwerela ku Galileya. ⁴ Koma chenzofunika kuti apitiletu mu Samariya. ⁵ Iye anangena mu komboni ya mu Samariya yamene inali kuitaniwa Sukari, iyi komboni, yenze pafupi na malo yamene Yakobo anapasa mwana wake wa chimuna Yosefe. ⁶ Chisime cha Yakobo chenzepo. Yesu anafuna kupumulako chifukwa ulendo unamulemesa. Ntawi yenze kuma 12. ⁷ Muzimayi waku Samariya anabwela kutapa manzi pamena paja pa chisime, Yesu anamuza ati, "iwe muzimayi nipaseko manzi nimwe." ⁸ Ndipo bopunzila bake sibenzepo chifukwa banabwelela mu komboni mukugulako vakudwa. ⁹ Manje muzimayi waku Samariya anayanka Yesu ati, "nanga nichani iwe wachi Yuda upempha manzi kwaine muzimayi wachi Samariya?" Chifukwa bantu ba Yudeya na bantu ba Samariya sibayendelana. ¹⁰ Yesu naye anamuyanka kuti, "sembe wenzekuziba mphase ya Mulungu, na wamene akuza ati 'nipase chakumwa,' sembe wamupempha, nayeve sembe akupasako manzi ya moyo wosasila." ¹¹ Muzimayi anakamba kuti, "Bambo, baketi yotapilako manzi mulibe, ichi chisime nichitali. Nanga manzi ya moyo muzayachosa kuti?" ¹² Sindiwe mukulu, mungamuchile tate wathu Yakobo, anatipasa chisime chamene ichi, nakumwamo eve pamozi nabana bake bamuna na vobeta vake?" ¹³ Yesu anayanka muzimayi ati, "wonse akumwa manzi yamene yachoka pa chisime ichi azanvela futi njota, ¹⁴ koma uyo wamene akumwa manzi yamene ine nipasa sazanvela njota futi. Ndipo manzi yamene nizamupasa yanzankala kasupe ka manzi mwayeve yo leta umoyo osasila." ¹⁵ Muzimayi anamuza kuti, "Bambo, nipaseni manzi yamene ayo nimweko pakuti, nisankanvele njota futi nileke kubwelanso kuno ku chisime mukatapa manzi masiko onse." ¹⁶ Yesu naye anamuyanka kuti, "iwe yenda ku nyumba kwako uyitane mwamuna wako, mubwele bonse kuno." ¹⁷ Muzimayi anamuyanka kuti, "nilibe mwamuna." Yesu anayanka kuti, "ndipo wakamba zoona kuti ulibe mwamuna, ¹⁸ chifukwa iwe unakwatiwapo ku ba muna bali 5, ndipo wamene uli naye apa simwamuna wako. Chamene wakamba ni chazoon." ¹⁹ Muzimayi anakamba kuti, "Bambo, naona kuti imwe ndimwe muneneli. ²⁰ Makolo batu banalambila pa luphiri apa, koma imwe mukamba ati ku Yerusalemu ndiye kumalo kwamene bantu bafunika kulambilila." ²¹ Yesu anamuza kuti, "nikulupilile ine, muzimayi, ntawi ibwela yamene simuzalambila Tate pa phili apa, kapena mu Yerusalemu. ²² Imwe mulambila chamena simuziba. Ife tilambila chamene tiziba, chifukwa chipulumuso chichokela kwa Ayuda. ²³ Koma, ntawi ibwela ndipo ntawi yafika, yamene bolambila ba zoona bazalambila batate mu muzimu na mu choonadi; chifukwa Batate basakila banthu basochabe kuti bankale womulambila. ²⁴ Mulungu ni Muzimu, ndipo bonse bolambila bafunika kulambila Ambuye mu muzimu na muchoonadi. ²⁵ Muzimayi anakamba kuli eve kuti "niziba kuti Mesiya abwela, (yamene aitaniwa Kristu). Akabwela azatipunzisa zintu zonse." ²⁶ Yesu anamuza kuti, "ndine wamene, wamene akamba naiwe." ²⁷ Pa ntawi yamene ija, wopunzila bake banabwelela. Manje banadabwa kupeza Yesu akamba namuzimayi, koma kulibe anakamba kuti, "nichani chamene ufuna?" kapena kuti "nanga nichani ukamba nauyu muzimayi?" ²⁸ Ndipo uyu muzimayi anasiya poto yake yamanzi nakubwelela ku komboni noyenda kuuza bantu kuti, ²⁹ "Bwelani, muone mwamuna wamene aniuza zonse zamene ninachita. Uyu sangankhale Kristu, angankhale?" ³⁰ Banachokamo mu komboni nakuyenda kwa eve. ³¹ Pantawi yamene ija, bopunzila bake benze kumulimbikisa kuti, "Mupunzisi, dyani." ³² Anabayanka kuti, "ine nili nachakudwa chamene inu bonse simuziba olo pang'ono." ³³ Bopunzila nawo bayamba kufunsana, "kulibe wamene amubwelesela chilichonse chakudwa, nanga bamuletela?" ³⁴ Yesu abauza kuti "chakudya changa nikuchita chifunilo cha eve wamene ananituma na kusiliza nchito yake. ³⁵ Kodi simumakamba kuti 'kwasala chabe myezi 4 kuti kukolola kuchitike?' Nikuuzani kuti nyamulani manso yanu nakuona minda, chifukwa minda yakonzekela ku kolola naku bweza va mu minda. ³⁶ Uyo wamena akolola amalandila malipilo yake, ndipo akututa mbeu ku moyo osasila, kuti ofesa na okolola akondwelee pamozi. ³⁷ Ndipo ichi chikamba kuti, 'wina afesa, wina akolola,' nicha zoona. ³⁸ Ine nakutumani kuti mukolole minda yamene simunalime. Benangu banasebenza, imwe mwangena chabe munchito yamene banzanu banasebenza kudala. ³⁹ Ba Samariya bambili mu muzinda uja banayamba kumukulupilila Yesu chifukwa cha umboni wamene enzekupasa muzimayi uja, kuti, "ananiuza vonse vamene ninachita." ⁴⁰ Pamene ba Samaliya banabwela kwa iye banamupempha kuti ayambe kunkala nabo, naye anankala nabo masiku yabili. ⁴¹ Na bambili banakulupilila chifukwa cha mau yake. ⁴² Banamuza muzimayi kuti, "sitinakhulupilile futi chifukwa cha mau yamene watuza, takhulupilila chifukwa cha mau yamene tazinvelea na mutu watu, ndipo taziba kuti uyu ni mupulumusi wa ziko lonse." ⁴³ Patapita masiku yabili, anachokako kuja nakuyenda ku Galileya. ⁴⁴ Chifukwa Yesu wamene anakamba kuti muneneli sibamupasa ulemu mu ziko yake. ⁴⁵ Pamene anangena mu Galileya, banthu bamu Galileya banamulandila bwino. Benze banaona zonse zama anachita kuja ku Pwando inankhalila ku Yerusalemu, chifukwa aba banthu nabo

benzeko ku Pwando yameni iyi. ⁴⁶ Anabwelelanso ku Kana ku muzinda wa Galileya, kwamene anasandusa manzi vinyo. Ndipo kunali mukulu wina wa ufumu, mwana wake anali odwala ku Kapernaumu. ⁴⁷ Pamene ananvela kuti Yesu achokako ku Yudeya nakubwela ku Galileya, anayenda kwa Yesu nakumupempha kuti abwele achilise uja mwana enze pafuti na kufa. ⁴⁸ Yesu anabauza kuti, "imwe ngati simunaone vizindikilo na vodabwisa, simuzakulupilila." ⁴⁹ Mukulu uyu anamuza kuti, "Ambuye imwe, bwelani kuno mwamusanga mwana wanga akalibe kufa!" ⁵⁰ Yesu anamuyankha kuti, "Yenda. Mwana wako ali namoyo." Mwamuna uyu anakulupilila zamene anakamba Yesu nakuyenda anayenda. ⁵¹ Akali kuyenda, ba nchito bake banakumana naye pa njila nakumuza kuti mwana wako ali namoyo. ⁵² Ndipo anabafunsa ntawi yamene mwana anachilisidwa, nabo banamuyanka kuti "anachilisidwa mailo na ntawi ya wanu koloko ya muzuba." ⁵³ Ndipo tate wamwana anazindikila kuti iyo nthawi yenze pamene Yesu anamuza kuti "mwana wako ali namoyo." Iye na banja yake yonse inakhulupilila mwa Yesu. ⁵⁴ Ichi ndiye chizindikilo chachibili anachita Yesu paneme anachoka ku Yudeya no yenda ku Galileya.

Chapter 5

¹ Pamene vinasila ivi penzeli chikondwewero cha Ayuda; ndipo Yesu anayenda ku Yelusalemu. ² Manje mu Yelusalemu pa geti ya mberere, mwenzeli mugodi wa manzi mu chiyebile benzo kaita ati Betesida, yenzeli namakholido yanamutenje yali faivi. ³ Mwamene umu munagona banthu bambili odwala, balibe menso, olemala nabozizila mendo kuyembekezela manzi yavundulike. ⁴ Mungelo wa Mulungu enzopitako nthawi zinangu kukavundula manzi, ndipo wamene angenamo pa festi manzi yakali yobvundulika enzo pola matenda yaliyonse yamene anali nayo. ⁵ Mudala winangu enzeli wodwala kwa zaka 38. ⁶ Pamene Yesu anamuwona kuti aligone, nobwela kuzindikila ati anankhalapo nthawi itali, anabwela amufunsa ati, ufuna kuti upolesewe? ⁷ Mudala uja odwala anabwela ayankha ati, "Ambuye, nilibe munthu oningenesa mu mugodi ngati manzi yavundulika. Nikafuna kungenamo, winangu abwela angenamo." ⁸ Yesu anabwela akamba ati "Nyamuka, tenga mphasa yako, yenda." ⁹ Pamene apo mudala uja anapola notenga mphasa yake, noyenda. Manje ija siku penzeli pa Sabbatha ¹⁰ So baYuda anabwela akamba namudala wamene anapola ati, "Lelo nipa Sabbatha, sufunka kunyamula mphasa yako." ¹¹ Anabwela ayankha ati, "Uja wamene wanipolesa waniuza kuti, 'Tenga mphasa yako yenda.'" ¹² Banabwela bamufusa ati, "Nindani mudala wamene akuuza kuti, 'Tenga mphasa yako, yenda?'" ¹³ Koma uja mudala anapolesewa sanamuzibe kuti nindani cifukwa Yesu anayenda yanoziba aliyense, cifukwa penzeli banthu bambili. ¹⁴ Pamene vinasila ivi, Yesu anamupeza yeve mu Tempele nobwela kumuuzi ati, "Ona, wapola manje! Usakacimwe futi, kuti coyipa cocila apo cisakacitike kuli iwe." ¹⁵ Mudala uja anayenda ndipo anauza baYuda kuti niYesu wamene anamucilisa. ¹⁶ Manje cifukwa ca ivi vinthu baYuda banamusausa Yesu, cifukwa cakuti anacita ivi vinthu pa Sabbatha. ¹⁷ Yesu anabwela abayankha ati, "baTate banga akali kusebenza namanje so, naine nisebenza manje so." ¹⁸ Cifukwa caici, baYuda anafunisisa kumupaya cifukwacakuti sanapwanye cabe siku la sabatha, koma anaitana Mulungu kunkhala Atate bake eve, nozipanga eve kulingana na Mulungu. ¹⁹ Yesu anabwela ayankha ati, "Nikuuzani coonadi kuti mwana Mwamuna sangacite vinthu payeve yeka, koma vamene awona baTate bake kucita, vonse vamene baTate acita, mwana mwamuna naive avicita. ²⁰ BaTate akonda mwana Mwamuna nakuti bamuwonesha vonse vamene bacita, nakuti bazamuwonesha vinthu vikulu maningi kucila apa ndipo muzadabwa. ²¹ Monga baTate bausha ba kufa nobapasa moyo, namwana Mwamuna apasa moyo kuli aliyense yeve afuna. ²² BaTate sibaweluza aliyense, koma apasa mwana Mwamuna kuweluzi konse ²³ kuti bonse balemekeze mwana Mwamuna mwamene alemekezela baTate. Wamene salemekeza mwana Mwamuna salemekeza baTate wake bamene anamutuma ²⁴ Kukamba zoonadi, yeve amene anvela mau anga nakukhulupira wamene ananituma anaumoyo wosasila ndipo kulibe ciweluzo, koma wacoka ku imfa wabwela ku moyo ²⁵ Kukamba zoonadi, nthawi ibwela, ndipo yabwela kudala, pamene bakufa bazanvela mau ya mwana Mwamuna wa Mulungu, ndipo amene azanvela azankhala na moyo. ²⁶ Monga mwamene baTate banamoyo mulibeve, bapasako futi namwana Mwamuna kuti ankhale namoyo muliyeve, ²⁷ nakuti baTate bapasa mwana Mwamuna ulamulilo kuti angapeleke ciweluzo cifukwa nimwana Mwamuna wa munthu. ²⁸ Osadabwa naici, ibwela nthawi pamene bonse bali mumanda wazanvela mau yake, ²⁹ ndipo bazacoka: baja bamene bacita bwino kukauka kwa moyo, baja bamene bacita zooipa kukauka ku ciwereluzi. ³⁰ Siningacite ciliconse paine neka. Pazamene nivela, niweluzi, ndipo ciweluzo canga nicolungama cifukwa sinicita mwamene nifunila ine koma nicita kulinga mwamene ananitumila. ³¹ Ngati nizakamba zaine neka, umboni wanga suzankhala wa zoonadi. ³² Koma kuli winangu amene apereka umboni wanga, ndipo niziba kuti umboni wamene apereka pali ine niwazoonadi. ³³ Imwe munatuma kwa Yohane, ndipo wapereka umboni wa zoonadi. ³⁴ Koma umboni wamene ndilandila siwucokela kumunthu. Nikamba vonse ivi kuti mupulumuke. ³⁵ Yohane anali nyali yoyaka nayowala ndipo imwe munafuna kuti mukodwela mukuwala kwake panthawi ing'ono cabe. ³⁶ Koma umboni wamene nili nabo upambana wa Yohane, pa zinchito zamene baTate bananipasa kuti nizikwanilise, zinchito zamene izi zamene nicita, zipoleka umboni kuti baTate bananituma ine. ³⁷ BaTate bamene bananituma ine bevebeka bapelekela umboni pazaine. Simunaveleko mau yabo kapena kubona vamenene abonekela. ³⁸ Mulibe namau yake yamene yankhala mwa imwe, cifukwa simukhulupilira muli iye wamene iye anatuma. ³⁹ Musakila mau aMulungu cifukwa muganiza kuti muliyeve muli umoyo bosasila, ndipo mau yamene aya yapereka umboni pali ine, ⁴⁰ ndipo simufuna kubwela kwa ine kuti mukhale nabo moyo ⁴¹ Sinilandila mayamiko kuchokela kubanthe, ⁴² koma niziba kuti mulibe cikondi ca Mulungu muli imwe. ⁴³ Nabwela muzina la baTate banga, koma simunilandila. Koma winangu akabwela muzinalake mungamulandile. ⁴⁴ Mungakhulupilile bwanji, imwe amene mulandila mayamiko kubanzanu koma simufuna kulandila mayimiko kuchokela kuli Mulungu aliyeka. ⁴⁵ Musanganize kuti ine nizakunenelani kuli baTate. Wamene akunenelani ni Mose, wamene mukhulupilira. ⁴⁶ Ngati mukhulupilira Mose, mungakhulupilire naine cifukwa Mose analemba zaine. ⁴⁷ Ngati simukhulupilira vamene analemba, mungakhulupilire bwanji mu mau yanga?"

Chapter 6

¹ Pathapita izi, Yesu anayenda kusidya kwa chimana ca Galileya, chochedwanso chimana ca Tibeliya. ² Gulu likulu la Anthu linamusata iye chifukwa linaona vodabwisa vimene anachita pa wodwala. ³ Yeso anakwela ku lupili nakhala pansi ndi wophunzila ake. ⁴ (Tsopano pwando, la Yuda ya pasaka, inali pafupi.) ⁵ Yeso anakweza maso naona gulu likulu la anthu ilikubwela kwa iye, ndipo anati kwa Filipo, "Tizagula kuti buledi kuti tidyese Anthu awa?" ⁶ (Koma Yesu anafunsa Filipo kumuyesa chabe, Chifukwa iye anaziwa camene ayenera kucita.) ⁷ Filipo anamuyankha nati, " Ngakale makobili miyanda iwili (200) kugula buledi singakwanila aliyense kuti adye ngakale kang'ono chabe. ⁸ M'modzi wa uphunzila ake, Andeleya mbale wa Simoni Petulo anati kuli Yesu, ⁹ "Alipo pano mnyamata aliko na buledi faive na nsomba ziwili, koma izi kulinganiza ndi anthu zingathandize?" ¹⁰ Yesu anati, " Awuzeni anthu ankhale pansi." (Panali uzu wambiri pamalo paja) Amuna amene anakhala pansi enzopitilila pa faive sauzande, (5,000). ¹¹ Yesu anathenga buledi atayamika anawapasa waja anakhala pansi Anachitanso chimodzi mozi ndi nsomba, anadya mwakufuna kwawo. ¹² Pamene banakhuta wonse iye anati kwa ophunzila ake, Tengani vasalapo kuti visaonongeke." ¹³ Conco iwo anasonkhanisa vesiyapo vakudya mabasiketi ya buledi twelufu kuchokela kuli faivi buledi yamene banadya. ¹⁴ Anthu pamene anaona chizindikilo chamene anacita anati, "Zoonadi munthu uyu ndi mneneli uyo amene akuza pa ziko lapansi." ¹⁵ Pamene Yeso anazindikila kuti afuna kumufaka pa ufumu, mwachikakamizo anachokapo nokwela ku lupili kwa yekha. ¹⁶ Pamene kwenzofipa mazulo, ophunzila ake anayenda ku chiimana. ¹⁷ Anakwela muboti noyambapo kuyenda kutauka chimana ku Kapenaumu. Kwenze kunafipa panthawi iyo, koma Yesu enze akalibe kubwela kuli beve. ¹⁸ Kwenze kunayamba chimphepho cikulu pa chimana nipo cinayofya. ¹⁹ Atayenda makilomita faivi kano sikisi, anamuona Yesu alikuyenda pa chimana alikubwela kufupi na boti, ophunzila anachita mantha. ²⁰ Koma Yesu anabauza, " Musachite mantha! ndine!" ²¹ Analola kumlandila mu boti, nthawi yomweyo boti inafika ku sidya uko kwamene benzoyenda. ²² Siku yokonkhapo, gulu likulu la anthu limene linali kuyembekeza kusidya kwina kwa chimana, anaona kuti kunalibe boti iliyonse koma cabe yamene ija Yesu sanangenemo na ophunzila ake, koma kuti ophunzila anayenda woka. ²³ Ndipo maboti yena yochokela ku Tibeliya anafika pafupi na pamalo pamene anadyela buledi ija ambuye anayamika. ²⁴ Pamene gulu la anthu linazindikila kuti Yesu na ophunzila wake sanalipo pamalo paja, anazitengela woka ma boti noyenda ku kapenaumu kukamufuna-funa Yesu. ²⁵ Pecimupeze kusidya ina ya chimana, anumufunsa kuti, "Rabbi munafika nthawi yanji kuno?" ²⁶ Yesu anayankha nati, "Zoonadi ndithu inu munifuna-funa kosati kuti munaona zizindikilo zodabwisa yai koma cikukwa munadya nokutha buledi. ²⁷ Katani nchito, kosati chifukwa cha vakudya voonongeka koma pavakudya vamene suvuonongeka mphaka kumoyo wosasila, vamene mwana wa Munthu azakupasani. Chifukwa Mulungu atate anasindikizya ndi chizindikilo chomuvomeleza." ²⁸ Ndipo anamufunsa iye nati, "Ticite chani kuti, tichite nchito ya Mulungu?" ²⁹ Yesu anayankha nati, "Nchito ya Mulungu ndi iyi; Khukulupilila muli yeve amene anatumiwa. ³⁰ Ndipo anamufunsa kuti, " kodi nga chizindikilo chodabwisa camene muzatipasa nicha bwanji kuti ife tikukhukulupilileni? Muchitepo ca bwanji?" ³¹ Makolo athu anadya manna m' chipululu, monga analembela malembo, " kuti anapasidwa buledi kucokela kumwamba kuti adye." ³² Yesu anayankha nati, "Zoonadi, senze Mose enze ekupasani buledi yofumila kumwamba koma ndi atate wanga wamene okupasani buledi yeni-yeni yochokela ku mwamba. ³³ Buledi ya Mulungu ndiye yocokela kumwamba, nopasa moyo ku chalo cha pansi." ³⁴ Nawo anamufunsa nati, "Ambuye, tipaseni buledi nthawi zyonse." ³⁵ Yesu anayankha nati, " Ine ndine Buledi wa moyo; aliyense azabwela kwaine sazamvela njala soti, nauyo ati anikhulupilire sazamvela njonta soti. ³⁶ Koma ndakuuzani kale, mwaniona koma simundikhulupilila. ³⁷ Aliwonse amene atate azanipasa azabwela kwa ine, nauyo wamene azabwela kwaine sindizamutaya konse. ³⁸ Chifukwa ndinaza ine kuchokela ku mwamba, kosati kuzocita chifunilo canga koma caiye amene ananituma ine. ³⁹ Ici niye chifunilo cauyo enituma cakuti nisataye ngakale umodzi wa iwo amene anandipasa iye, koma kuti nikawause pa siku yomaliza. ⁴⁰ ici ndiye chifunilo cha Atate, kuti aliyense waona Mwana nomukhulupirila ankhale ndi moyo wosata, ndipo ndizamuusa kwa akufa pa siku lomaliza. ⁴¹ Pamenepo Ayuda anayamba kung'ung'uzila chifukwa anati, " Ine ndine buledi wocokela ku mwamba." ⁴² Anati, " Si Yesu uyu mwana wa Yosefe, Mayi ake ndi Abambo wake timawaziba? bwanji akamba ati, ine ndinachokela ku mwamba?" ⁴³ Yesu anayankha anati, "musang'ug'uze mweka-mweka. ⁴⁴ palibe munthu angabwele kwa ine ngati Atate anandituma sanamubwelese kwanga, ndipo ndizamuusa kwakufa pa siku yomaliza. ⁴⁵ Zinalembedwa ndi aneneli, 'wonse azaphunzidwa ndi Mulungu' Aliwonse amene amamva ndi kuphunzira kwa Atate amabwela kwa ine. ⁴⁶ Palibe amene anamuonapo Atate, kuchoselako chabe uyo anachokela kwa Mulungu yekhayo ndiye anaona Atate. ⁴⁷ Zoonadi yense amene akhulupirila alinawo moyo wosatha. ⁴⁸ Ine ndine buledi wa moyo. ⁴⁹ makolo anu anadya mana mchipululu, ndipo anafa. ⁵⁰ Buledi yamene unachokekela kumwamba, kuti munthu aliyense akadyako sazafa. ⁵¹ Ndine buledi wa moyo wamene inachokele

ku mwamba. Ngati wina wadyako buledi iyi azakhala na moyo nthawi zonse. Buledi yamene nikupasani ni thupi yanga kuti anthu pa dziko lapansi akhale ndi moyo." ⁵² Ayuda anaphya mtima noyamba kutsutsana kwambili pakati pawo kuti, "Uyu munthu angatipase bwanji thupi yake kuti tidye?" ⁵³ Yesu anayankha nati, "Zoonadi ndikuuzani ine ngati simukudya thupi la Mwana wa Munthu ndi kumwa mlopa wake simuzankhala na moyo mwaimwe. ⁵⁴ Aliwonse azadya thupi yanga nakumwa magari yanga, azankhala na moyo wosatha, ndipo ndizamuusha pa siku yosiliza. ⁵⁵ Pakuti thupi langa ndi chakudya cheni-cheni ndi magari yanga ndi Chakumwa cheni-cheni. ⁵⁶ Iye amene azadya thupi langa ndi kumwa magari yanga azankhala mwa ine ndi ine mwa iye. ⁵⁷ Monga Atate wa moyo ananituma, ndipo ndili ndi moyo chifukwa cake aliyense amene azadya ine azakhalanso ndi moyo chifukwa ca ine. ⁵⁸ Iyi ndiye buledi yamene yochokela ku mwamba, osati ija yamene anadya makolo yathu nakufa. Iye amene azadya buledi iyi azakhala ndi moyo wosatha." ⁵⁹ Yesu analankhula zinthu izi pamene anali kuphunzitsa musunagoge mu kapanawo. ⁶⁰ Ambiri ophunzila bake pamene anamvwa izi anati, "Ici ndichiphunzitso chovuta ni ndani angacivomele?" ⁶¹ Yesu, pozindikila mwaiye yeka kuti ophunzila bake alikung'ung'onzila, anawafunsa nati, "ivi vakukalipisani?" ⁶² Manje nanga mukazaona Mwana wa Munthu akukwela kumene anachokela! ⁶³ Mzimu apasa moyo, thupi siipindulapo kanthu. Mau amene nakamba namwe ni mzimu ndipo ndi amoyo. ⁶⁴ Alipo ena aimwe amene simukhulupilila, "Yesu anazindikila kuyambila pachiyambi amene samkhulupirila ndi amene azamugulisa. ⁶⁵ Iye anati, "Ndichifukwa chake ndinakuuzani kuti palibe amene azabwela kwa ine pokhapo Atate andipasa iye kwa ine. ⁶⁶ Chifukwa ca ici ambiri wophunzila ake anabwelela sanayendenso na iye. ⁶⁷ Ndipo Yesu anati kuli aja ena twelufu ati, "Naimwe mufuna kubwelela, kodi muyende? ⁶⁸ Sayimoni Petulo anayankha, "Ambuye tizayenda kuti? muli ndi Mau ya moyo wosatha. ⁶⁹ Ndipo tazindikila, takhukulupirila kuti ndinu Woyela wa Mulungu." ⁷⁰ Yesu anati kwa iwo, "Sindine wamene ndinakusankhani twelufu? Koma umodzi wa imwe ndi satana. ⁷¹ Apo anali kunena Yudasi mwana wa Sayimoni Isikariyoti, ndiye wamene anagulisa Yesu.

Chapter 7

¹ Ndipo zitapita izi Yesu anayendayenda m'galileya; pakuti sanafune kuyendayenda m'yudeya cifukwa ayuda anafuna kumupha iye. ² koma phwando la yuda, phwando lamisasa, linayandikira. ³ Cifukwa abale bake anati kwaiye, 'chokani pano muyende, ku yudeya kuti ophunzila banu akapenye nchito zanu zimenemucita. ⁴ Pakuti palibe munthu acita kanthu mobisika, nafuna yekha kukhala poyera. Ngati muchtita izi ziwoneseleni ime mweka ku diziko lapansi. ⁵ Pakuti angakhale abale bake sanakhulupirira iye. ⁶ Cifukwa chake Yesu ananena nao, Nthawi yanga siinafike, koma nthawi yanu niyokonzeka masiku onse. ⁷ Dziko lapansi silingathe kudana ndi inu; koma ine inizonda kamba kakuti ine nimaichitila umboni, kuti nchito zao ni zonyansa, ⁸ Endan kuphwando; sinibwelako ine kuli iyi yamanje apa; pakuti nthawi yanga siinafike. ⁹ Ndipo m'mene adanena nao zimenezi anakhala m'Galileya. ¹⁰ Koma pamene abale bake anakwela kuyenda kuphwando, pomwepo iyenso anakwela, si poonekera, koma monga mobisika. ¹¹ Ayuda analikumfuna iye paphwando, nanena, ali kuti uja? ¹² Ndipo kunali vokamba kamba pali iye m'mubanthu, ena ananena, kuti ali bwino; koma ena ananena iyai, koma asochelesa banthu bambili. ¹³ Nangu kuti banakamba vonse ivi panalibe munthu anakamba za iye poyera, cifukwa ca kuyopa Ayuda. ¹⁴ Koma pamene phwando inafika pachimake, Yesu nalowa mutepele, naphunzitsa. ¹⁵ Ayuda anadabuwa, nanena, aziba bwanji zolemba, wosaphunzira? ¹⁶ Pamenepo Yesu anayankha iwo, nati, "Chiphunzitso sichanga koma nichawamene ananituma ine. ¹⁷ Ngati munthu aliyense afuna kucita chifuniro chake, adziba za ciphunzitso, ngati cicokera kwa Mulungu, kapana nikamba zocokera kwa ine. ¹⁸ Iye wolankhula zocokera kwa iye yekha afuna ulemu wa mwini yekha, iye wakufuna ulemu wa iye amene anamtuma, iye ali woona, ndipo mwa iye mulibe cosalungama. ¹⁹ Si Mose kodi anakupasani lamulo? kulibe munthu pali imwe kusunga lamulo. Mufuna kunipaya cifukwa? ²⁰ Khamu la anthu linayankha, Muli ndi ciwanda afuna ndani kukuphani? ²¹ Yesu anayankha kwa be eve, Ndinacita nchito imozi, ndipo munadabwa ²² Monse anakupasani mdulidwe (si ucokera kwa Mose, koma kwa, makolo), ndipo mudula munthu tsiku la Sabata. ²³ Ngati muthu alandila mdulidwa tisku la Sabata, kuti cilamulo ca Mose cingapasulidwe; ninshi chamene munikwiira ine nichaini? cifukwa nachilisa munthu tsiku la Sabata? ²⁴ Musaweruze monga maonekedwe, koma weruzani ciweruziro chazoon. ²⁵ Pamenepo ena a iwo a ku Yerusalemu ananena, siuyu amene afuna kumupha? ²⁶ onani, akamba poyera, ndipo sanena kanthu kwa iye. Sichinga kale kuti oweluzi adziwa ndithu kuti ndiye Kristu wamene, si so? ²⁷ Koma ameneyo tidziwa uko acokera; koma Kristu pamene azabwela, palibe ummodzi adzaziwa uko acokera. ²⁸ Pamenepo Yesu anafuula mutepele, alikuphunzitsa ndi kunena, Muniziba ine, ndiponso mudziwa kwamene nicokela, sindinabwele ine neka, koma iye anituma ine amene inu simumziwba, ali woona. ²⁹ Ine nimuziba iye; cifukwa ndine wocookera kwa iye, ananituma ine. ³⁰ Pamenepo anayesa kumgwira iye; koma palibe wamene anamgwira kumanja, cifukwe nthawi yake siinafike. ³¹ Koma ambiri a mkhamu la anthu anakulupirira iye; ananena, "pamene Kristu akadza kodi adzacita zizindikilo zambiri zoposa zimene adazicita?" ³² Aye farisi anamva khamu la anthu belabelasa za Yesu; ansembe, akulu ndi Afafrisi anatuma ashylika kuti akamgwira. ³³ Yesu anati, Kasala kanthawi nili naimwe, ndipo niyenda kwa eve wonituma ine. ³⁴ Mudzafunafuna ine, osandipeza; ndipo kwamene niyeda, inu simungathe kubwelapo. ³⁵ Cifukwa chake Ayuda anati mwa iwo okha, azakayeda kuti uyu muthu kuti ife sitingamupeze? adzamuka kwa Bagreek obalalikawo, ndi kuphunzitsa Bagreek? ³⁶ Mau awa amene ananena ndi chiani, Mudzadifunafuna osandipeza; ndipo pomwe ndiri ine, inu simungathe kunipeza?" ³⁷ Koma tsiku losiliza, lalikuru la phwando, Yesu anaimiria nakupunda, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva njota, abwele kuli ine namwe. ³⁸ eve wokhulupirira ine, monga malembo anati, misinje ya madzi amoyo azayende, kuchoka mumala mwake. ³⁹ Koma ici ananena za Mzimu, amene iwo akukhulupirira iye anati adzalandire; pakuti Mzimu sana pasiwe pamenepo, cifukwa Yesu sanalemekezedwe. ⁴⁰ enangu muchigulu pakumvela mau, ananena, amene uyu ni m'neneri, ⁴¹ Ena ananena, uyu ndiye Kristu, Koma ana ananena kodi Kristu azachokela mgalileya? ⁴² Kodi siyanati malembo kuti Kristu azacokela mubanja ya David ndi Betelehemu muzi mwenze David? ⁴³ Munahuka kusiyana m'gulu cifukwa ce iye. ⁴⁴ Koma ena mwa iwo anafuna kumgwira iye, koma palibe muthu anamgwira mo. ⁴⁵ Pamenepo kunabwela asilikali kwa akulu ansembe ndi Afarisi, ndipo amena aba anati kwa beve, nichani simunamulete? ⁴⁶ Asilikali anayankha, palibe munth analankhula coter. ⁴⁷ Pamenepo Afarisi anayankha iwo, kodi mwasokeretsedwa inunso? ⁴⁸ kodi wina wa akuru wa khulupirira mwa iye, kapenawa Afarisi? ⁴⁹ koma gulu ili losaziwa malamulo, likhala lotembereledwa. ⁵⁰ Nicodimo umozi wa Afarisi (amene anabwela kwa Yesu poyamba) anati kwabeve ⁵¹ Kodi malamulo athu apeleka chiweruzo ku munthu osayamba kumvela kulieve noziba cimene, acita? ⁵² Anyankha nati kwa iye, kodi iwenso uli woturuka mGalileya? funafuna, uoni kuti m'Galileya sikungacoke mneneri. ⁵³ Ndipo anayenda munthu yense ku nyumba yake.

Chapter 8

¹ Yesu anayenda kupili ya oliva. ² Kuseni- seni anabwela ku tempele nafuti, ndipo banthu bonse banabwela kwa eve; ndipo anakhala pansi nakubapunzisa. ³ Balembe na bafalisi banabwelesa mukazi banagwila achita chigololo ndipo anamuimika pakati. ⁴ Ndipo banamuza kuti, muphunzisi, mukazi uyu bamugwila achita chigololo. ⁵ kulingana namalamulo, Mose anatilamulila kuti banthu monga aba tibateme myala kuti bafe; mukamba chani pali uyu?" ⁶ Banakamba ivi kuti bamuyese nzeluzake, koma Yesu anabenda pansi nakulemba nachikumo chake pansi. ⁷ Pamene anapitiliza kumufusa mafunso, anaimilila na kukamba kuti, wamene aliye chimo, ankhale oyamba kuponya mwala uyu." ⁸ kachibili anabenda pansi nakulemba pansi kachibili. ⁹ Pamene banamvela, banayamba kuchokapo umozi umozi, kuyambila bakulu. Posiliza Yesu anasala yeka, na mukazi anali pakati pawo. ¹⁰ Yesu ananyamuka nakumufunsa mukazi, "bali kuti bamene bakunamizila? nanga pali bamene bakususa?" ¹¹ Mukazi anakamba kuti. Yesu anakamba kuti naine sinikususa. Yenda wusakachimweso. ¹² Nafuti Yesu anabauza kuti, "Ndine kuunika kwa ziko; wamene azanikonka sazayenda mumudima koma azankahala na nyali yamoyo." ¹³ Bafalisi banamuza kuti, "upelekela umboni pazaiwe weka; umboni wako siwazoon." ¹⁴ Yesu anabayanka kuti, "Ngankale nipase umboni paine neka, umboni wanga niwazoon. Niziba kwamene nichokela nakwamene niyenda, koma simuziba kwamene nickokela na kwamene niyenda." ¹⁵ Muweluzi monga mwathupi; ine siniweluzi aliyense. ¹⁶ Koma ngati naweluzi, ku weluzi kwanga ni kwazoon chifukwa sinili neka, koma, nili na baTate bananituma. ¹⁷ Zoon, na mumalamulo yanu chinalebwa kuti umboni wa banthu babili niwa zoon. ¹⁸ Ine ndine wamene nichita umboni pa ine neka, ndipo Batete bananituma banichitila umboni wanga." ¹⁹ Banamuza kuti, Batate bako bali kuti? Yesu anayankha, simuziba aTate nainenso simuniziba; ngati kuti munali kuniziba, sembe munabaziba naba Tate banga." ²⁰ Anakamba mau aya, mu nyumba yosungilamo chuma mukachisi, Ndipo palibe anamumanga, chifuka nthawi yake siinafike. ²¹ Anakamba nafuti kuli beve, "Ine niyenda; muzanifuna ndipo muzafa mumachimo yanu. Kwamene niyenda, simungabweleko." ²² Bayuda banakamba kuti, kansi azazipaya yeka? Nanga ndiye chamene akambila kuti, ' kwamene niyenda simunga bweleko?" ²³ Yesu anati kuli beve, "muchokela pansi; ine nichokela kumwamba. Ndimwe ba paziko; Sindine wapaziko lapansi. ²⁴ Chifukwa chaichi, ninakaba kuti muzafa mumachimo yanu. Koma mukakhulupilila kuti INE NDIYE WAMENE, muzafa mumachimo yanu. ²⁵ Pamenepo ananena kwa iye, "Ndiwe ndani?" Yesu anati kwa beve, "Pazamene nakamba kuchokela pachiyambi. ²⁶ Nilinazambiri zokamba ndi kuweluzi pali imwe. koma, lye ananituma ni wazoon; ndipo zhintu zamene ninamvela kuchokela kwa yeve, izi zinthu nikamba kuziko lapansi." ²⁷ Sibananvese kuti anali kukamba nabeve pali za Batate. ²⁸ Yesu anakamba kuti, "Pamene munyamula mwana wa munthu, ndiye pamene muzaziba kuti NDINE, ndipo sindichita chilichose kwaine neka. Monga Atate ananiphunzisa, nikamba ivi vinthu. ²⁹ Wamene ananituma ali naine, ndipo sananisiye neka, chifukwa nthawizonse nimachita zomukondwelesa." ³⁰ Pamene Yesu analikukamba vinthu ivi, bambili banakhulupilila. ³¹ Yesu anakamba kuli Bayuda baja bamene banamukhulupilila, "Ngati munkhala mu mau yanga, ndipo muzankala opunzila banga; ³² Ndipo muzaziba choonadi, na choonadi chizakumasulani." ³³ Anamuyanka kuti, "Ndife mubadwo wa Abrahamu ndipo sitinankhalepo bakapolo ba aliyense; ungakambe bwanji; muzamasulidwa?" ³⁴ Yesu anayankha kuti, "Zoon, Zoon, nikuuzani kuti, aliyense wamene achita uchimo ni kapolo wa chimo. ³⁵ kapolo sankhalilila munyumba muyayaya; mwana ankhaliilila muyayaya. ³⁶ Mwaichi, ngati mwana akumasula, uzamasuliwa vazona. ³⁷ Niziba kuti ndimwe mubadwo wa Abrahamu; koma mufuna kunipaya chifukwa mau yanga yalibe malo mwa imwe. ³⁸ Nikamba zimene naona mwa batate, ndipo mumachita vamene munavela kuchoka batate banu." ³⁹ Banamuyanka na kumuza kuti, "batate bathu niba Abrahamu, "Yesu anabauza kuti, " ngati mwenzeli bana ba Abrahamu, mungachite ntchito za Abrahamu. ⁴⁰ Koma, manje mufuna kunipaya, munthu wamene anakuuzani choonadi chimene ninavela kwa Mulungu. Abrahamu sanachichitete. ⁴¹ Muchita ntchito ya batate banu." Banamuza kuti, "sitinabadwe muchigololo; tili naye Tate umozi: Mulungu." ⁴² Yesu anabauza kuti. "Ngati mulungu anali Tate wanu, sembe munikonda, pakuti nichokera kwa Mulungu ndipo nili pamene pano; sininabwele pali ine neka. ⁴³ Koma ananituma. Chifukwa nichani simumvesesa mau yanga? Nichifukwa simunvela mau yanga. ⁴⁴ Ndimwe baba tate banu, mudielekezi, ndipo mufuna kuchita zofuna za batate banu. Anali wopaya kuchokela pachiyambi ndipo saimilila muchoonadi pakuti muli eve mulibe choonadi. Pamene akamba boza, akamba kuchokela ku chinkhalidwe chake chifukwa niwaboza ndipo ni tate wamaboza. ⁴⁵ Koma, chifukwa nikamba va zoon, simunikhulupilila. ⁴⁶ Nindani pali imwe anipeza nachimo? Ngati nikamba chazona, nichifukwa chani simunikhulupilila? ⁴⁷ Wamene ali wa Mulungu anvela mau ya Mulungu; simuyavela mau chifukwa sindimwe ba Mulungu." ⁴⁸ Bayuda banamuyakha kuti, "Sitikamba zoon kuti ndiwe Msamaria nakuti uli nachibanda?" ⁴⁹ Yesu anayankha, "nilibe chibanda, koma nilemekeza baTate banga, ndipo imwe simunipasa ulemu. ⁵⁰ Sinisakila ulemeleo wanga; aliko wina asakila na kuweluzi. ⁵¹ zoon, zoon, nikamba kuli imwe, ngati

wina asunga mau, sazaona imfa." ⁵² Ayuda banamuuza kuti, "Tiziba manje kuti uli na chibanda. Abrahamu na baneneli banafa; koma ukamba, ngati aliyense asunga mau yanga sazaona imfa; ⁵³ Sindiwe wamkulu kupambana atate bathu Abrahamu wamene anafa, nanga ndiwe mukulu? Baneneli nabonso banafa. Uzipanga kuti ndiwe ndani? ⁵⁴ Yesu anayanka, "ngati nizilimekaza neka, ulemelelo wanga ulibe nchito; niba Tate banga bamene bamanilemekeza -abo bamene mukamba kuti Mulunga wanu. ⁵⁵ Simunamuzibe yeve, koma nimuziba. Ngati nizakamba kuti; sinimuziba yeve; nizankhala monga imwe, baboza. Koma, nimuziba ndipo nisunga mau yake. ⁵⁶ Batate banu ba Abrahamu banakondwela pakuona siku yanga; banayiona ndipo banasangala." ⁵⁷ Ayuda anati kwa lye, "Mukalibe kukwanisa zaka 50, ndipo mwamuona Abrahamu?" ⁵⁸ Yesu anabauza kuti, "Zoona, zoona, nikamba kuli imwe, pamene akalibe kunkhalako Abrahamu, INE NDINE." ⁵⁹ Pamenepo banetenga myala kuti bamuteme nazo, koma Yesu anazibisa nochokamo mu Tempele.

Chapter 9

¹ Manje pamene Yesu analikupita, anaona mwamuna wamene sanali kuona kuchokela pamene anabadwila. ² Bopunzila bake banamufunsa kuti, Mupunzisi, nindani anachimwa, pakati pali uyu mwamuna na makolo bake, kuti abadwe osaona?" ³ Yesu anayanka kuti, uyu mwamuna sanachimwe, kapena makolo bake, koma kuti zinchito za Mulungu zioneke muli iye. ⁴ Tifunikila kuchita zinchito zake kukali muzuba, chifukwa usiku ubwela pamene sitizasebenza. ⁵ Pamene nilimuziko, ndine nyali yaziko. ⁶ Pamene Yesu anasiliza kukamba ivi vinthu, anatunya mata padoti, nakupanga matika ya mata, nakumuzoleka mumenso. ⁷ Anamuza, "yenda, ukasambe mu musinje wa siloam" [itatana uza kuti "kutumiwa"]. Mwamuna uyo anayenda, mukusamba, nakubwela ayangana. ⁸ Bantu banakala na'uyu mwamuna anali mpofu pafupi, nabamene banamuziba ati niwo pempa pempa banali kukamba kuti, "si'uyu mwamuna, anali kunkala nakupempa?" ⁹ Bena banali kukamba kuti, "niwamene". Bena banakamba kuti, "Iyai, koma alimonga eve". Koma anakamba kuti, 'ndine'. ¹⁰ Banakamba kuli iye, "nanga menso yako yanavulika bwanji?" ¹¹ Anayanka, "mwamuna oyitanidwa Yesu, anapanga matika yama mata nakunizoleka mumanso nakuniuza," yenda ukasambe ku siloam. ¹² Ninayenda mukusamba, pamene menso yanga yanavulika. ¹³ Banakamba kuli iye, "alikuti?" Anayanka, "siniziba." ¹⁴ Banaleta wamene enze mpofu kwa Afarisi, ¹⁵ Koma inali siku ya sabatha yamene Yesu anapanga matika nakuvula manso yake. ¹⁶ Pamenepo afarisi anamufunsa mwamene menso yake anavulikila. Anabayanka, "Anafaka matika mumenso yanga, ninayenda kusamba ninayangana. ¹⁷ Afarisi bena banati." Uyu mwamuna sanachokele kuli mulungu, chifukwa sasunga sabata. ¹⁸ Bena banati, "Nanga muntu ochimwa angachite bwanji vodabwisa?" Kunankala kugabanikisa muntu ndi muzake. ¹⁹ Banamufunsanso wamene enzeli mpofu, "Ungakambepo shani pali uyu muntu chifukwa anakuvula menso?" Anali mpofu anayanka kuti, "Nimuneneli." ²⁰ Cifukwa cace ayuda sanakhululupire za iye kuti anali mpofu kufukila kumene anayitana makolo bake bauja enze mpofu. ²¹ Banafunsa makolo bake, "Uyu ndiwe mwana wanu wamene anali mpofu? Nanga avulika bwanji menso?" ²² Makolo bake banayanka, "Tiziba ati uyu nimwana watu ndiponso anabadwa mpofu. ²³ Mwamene aonela, sitiziba, nawamene amuvula menso, sitiziba. Mufunseni, nimukulu. Angazikambile." ²⁴ Makolo ake anankamba izi zinthu, cifukwa enzekuyopa ayuda, Cifukwa ayuda anavomekesa kudala kuti ngati muntu alionse wamene azakamba ati niyesu, bazamuponya panja pa synagogo. ²⁵ Cifukwa cayici, makolo bake banati, "Nimukulu, mufunseni." ²⁶ Pantawi yacibili banaitana uja mwamuna enze mpofu nakumu'za, "Pasa ulemelelo kulimulungu." ²⁷ Tiziba ati uyu muntu niwocimwa." ²⁸ Uja muntu anayanka, "Siniziba ngati niwocimwa. Cintu cimozi chamene niziba: Nenze mpofu, koma lelo nalangana." ²⁹ Banamu'za, Anacita cani kuli iwe? Anavula bwanji manso yako?" ³⁰ Anayanka, "Naku'uzani kudala, manje simunanvele! Nicani mufunakuziba futi? Simufuna kunkala bopunzila bake, mufuna?" ³¹ Banamutukana nakukamba ati, "Ndimwe bapunzisi bake, koma ise ndise bapunzisi ba Mose. ³² Tiziba kuti mulungu anakamba na Mose, koma sitiziba kwamene uyu acokela." ³³ Banamutukwana nakukamba kuti, "Ndiwe opunzila wake, koma ise ndise opunzila ba Mose. ³⁴ Tiziba kuti Mulungu anakamba naye Mose, koma uyu eve sitiziba kwamene anachokela. ³⁵ Mwamuna anayanka nakubauza ati, "Ici nichozibika, kuti siniziba nakwamene acokela, koma ananivula manso. ³⁶ Tiziba kuti mulungu samanvela bocimwa, koma ngati niwozipoleka ndipo ama cita cifunikilo cake, amamunvela. ³⁷ Kucokela kuciyambi ca ziko kunalibe kuvekako ati muntu anabadwa mpofu avulika manso. ³⁸ Ngati uyu muntu sanacokele kuli mulungu, ngasanacitepo vilivonse." ³⁹ Banayanka nakumu'za uyu mwamuna, "Unabadwa mucimo, ndipo utipunzisa?" Cinakonkapo banamutaya panja. ⁴⁰ Yesu ananvela kuti banamutulusa mu synagogo. Anamupeza nakumu'za, "kodi unakululupila muli mwana wa muntu?" ⁴¹ Anamuyanka nakuti, "Nindani, mulungu, kuti nikululupile muli iye?" ⁴² Yesu anamu'za, wamuona, ndipo niwamene akamba naiwe." ⁴³ Mwamuna anakamba, "Ambuye, nakululupila" ndipo anamumpempeza. ⁴⁴ Yesu anati, "Mukuwelusa nicamene nina bwelela muziko kuti bonse abo bamene sibalangana balangane nabonse abo bamene balangana bankale mpofu." ⁴⁵ Afarisi bena banali naye bananvela vintu nakumufunsa, "Nanga naise ndise mpofu?" ⁴⁶ Yesu anakamba nabo, "Ngati munali mpofu, ngati mulibe cimo, koma apa mukamba, Tilangana; ndipo cimo yanu isala.

Chapter 10

¹ Indetu indetu ndinena kwainu wamene sangenela pa kageti koma angena chokwela pamwamba pa yakhola nikawalala kapena wachifwamba. ² koma wamene angenela pakhomu ndiye mubusa weniweni wankhosa. ³ Osunga khomo amusegulila eve. Nkhosa zimvela mau ake ndipo mubusa aitana nkhusa zake na mazina yake. ⁴ pamene wachosa nkhusa, azisogolela komanso zimulondola chifukwa zimvela mau ake. ⁵ nkhusa sizilondola mulendo koma zimuthaba, chifukwa ziziba mau ya mulendo. ⁶ Yesu anabauza Nthano iyi koma sanamvesese zinthu zamene analikulankhula kuli beve. ⁷ Yesu anati kwa iwo indetu indetu ndinena kwa inu, ine ndiye khomo lankhosa. ⁸ Aliyense wamene abwela pambuyo panga nikawalala ndipo nkhusa sizinamvele mau ache. ⁹ Ine ndine khomo, aliyense amane alobela pali ine azapulumusidwa, azalowa nakutuluka ndipo azapeza musipu. ¹⁰ Kawalala amabwela na lingo ya kuba, kupha ndikuononga. ine ninabwela kuti akhale nao umoyo wochuluka. ¹¹ Ine nine mubusa wabwino, ndipo mubusa wabwino apeleka umoyo wake ku nkhusa zake. ¹² Kapolo olembedwa ntchito sakhala mubusa chifukwa alibe Nkhosa. akaona mimbulu ibwela amasiya nkhusa zake nakuthaba. ndipo mimbulu imatenga nkhusa nakuzimwazya. ¹³ Iye amathawa chifukwa nikapolo wamene analembedwa chabe ntchito ndipo sasamalila Nkhosa. ¹⁴ Ine ndine mubusa wabwino, niziba nkhusa na nkhusa ziniziba. ¹⁵ Atate aniziba nainenso niziba atate chifukwa nipeleka umoyo wanga monga nsembe ku nkhusa zanga. ¹⁶ Nilinazo nkhusa zinangu zamene sizichokela mukhola iyi. Nizazibwelesa mukhola kuti zinkhale pamozi, zimvela mau aga ndipo zizakhala zimozi na mubusa umozi. ¹⁷ Ichi ndiye chifukwa chake atate banga banikonda chifukwa nimapeleka umoyo wanga nakuutenga futi. ¹⁸ Kulibe wamene atenga umoyo wanga koma ine neka niupeleka kunkhosa. Nilinawo ulamulilo wopeleka umoyo wanga komanso nikuutenga. Iyi nilamulo yamene ninalandila kuchokela kwa atate. ¹⁹ Mukangano unauka pakati pao pamene amvela mau aya. ²⁰ Bambili anayamba kuti uyu alina dimoni komanso niwofuntha. Kodi nichiani mumumvelela? ²¹ Bena banakamba kuti aya siyangankhale mau ya Dimoni. Kodi Dimoni Ingakwanise kusegula menso ya munth wakhungu? ²² Ndipo iyi inali nthawi ya madyelelo yo peleka kachisi, ²³ Inali nthawi ya mphepo ndipo Yesu anali kuyenda yenda mu Tempele ya solomo. ²⁴ Ndipo Ayuda anamuzungulila nakuyamba kumufunsa kuti "kodi nichani tiuziletu poyera kuti tikhulupilile, Kodi ndiwe Mesiya? ²⁵ Yesu anabayankha, Namuuzani koma simukhulupirila. Zintchito zamene nichita muzina la atate zinichitila umboni ine. ²⁶ Koma simukhulupilila chifukwa sinimwe nkhusa zanga. ²⁷ Nkhosa zanga zimvela mau anga ndipo niziziba elo zimanilondola. ²⁸ Nimazipasa umoyo wosatha ndipo sizizafa ndipo kulibe azazichosa kuli ine. ²⁹ Atate amene ananipasa nkhusa izi nimukulu kuchila onse ndipo kulibe wamene angazichoseko kuli Atate. ³⁰ Ine ndi Atate ndise bamozi ³¹ Ndipo Ayuda anatenga myala kuti amteme yeve. ³² Yesu anati Nakuonesani nchito zambiri kuchokela kuli Atate, mufuna muniteme myala panchito ziti? ³³ Ayuda anati sitizakutema myala patchito zabwino zamene wachita koma pa kunyozela mulungu pamene wazipanga kunkhala mulungu. ³⁴ Yesu anabayankha, sichinalembedwa kuti "Ninanena kwainu kuti ndinu milungu, ana a Mulungu waphamvu zonse. ³⁵ Ngati anabaitana milungu kwamene mau yanabwelela(ndipo malembo siyangapwanyike.) ³⁶ Kodi mukamba bwanji kuli wamene Mulungu anatuma kubwela muziko kuti "Unyozela Mulungu" Kamba kakuti namuuzani kuti ndine mwana wa Mulungu. ³⁷ Ngati sinichita nchito ya Atate musanikhulupilile, ³⁸ koma ngati nichita ntchito za Mulungu olo kuti simukhulupilila ine, khulupililani muntito kuti muzindikile naku mvesesa kuti Atate alimwaine ndipo ine nilimuliyeye. ³⁹ Anayesa kuti amuchite chifwamba koma anachoka mumanja yao. ⁴⁰ Anapitanso kuja ku Yolodani kwamene Yohane anali kubatiza banthu ndipo anakhala kwamene kuja. ⁴¹ Bambili banabwela kuliyeye nakumuza kuti Yohane sanachite miraculi iliyose, koma vilivonse vamene Yohane anakamba pali uyu munth nivazoon. ⁴² Bambili banamukhulupilila kwamene kuja.

Chapter 11

¹ Koma panali munthu wodwala, Lazaro wa ku betaniya, wa m'muzinda wa Mariya ndi mbale wake Marita. ² koma ndi Mariya wamene anadzoza Mbuye ndi mafuta onunkhira bwino ndiponso anapokuta mendo yake na sisi zake, amene mbale wake Lazaro anali odwala. ³ Aba abale anaitana Yesu, nakukamba kuti, "Mbuye, onani, iye wamene mukonda adwala." ⁴ pamene Yesu ana mvela izi, anakamba kuti, "ayamatenda siyo peleka ku infa, koma ni ku ulemelelo wa Mulungu kuti mwana wa Mulungu aka lemekezedwe pali ichi. ⁵ Koma Yesu anakonda Marita ndi Mariya na Lazaro. ⁶ pamene ana mvela kuti Lazaro ni odwala, Yesu anankhalako masiku awili kumalo kwamene analili. ⁷ koma kuchokela apa, anakamba ku ophunzira bake, "Tiyeni tiyende ku Yudeya nafuti." ⁸ Aba ophunzila anakamba, "Aphunzisi, apa manje ayuda ayeselela kuku lasani myala, muyendako futi?" ⁹ Yesu anayanka, "kodi simuli ma awala kumi imozi ndi awiri mukuunika kwa siku? ngati wina wake aendela mu ntawi ya siku, sizazibuntula, chifukwa aona na nyali ya zikolino. ¹⁰ Koma, ngati munthu ayenda usiku, azazibuntula chifukwa nyali si ili muli iye." ¹¹ Ndipo anakamba zinthu, kuchokela izi zinthu, Anakamba kuli bemve, "mubale watu Lazaro agona mutulo, koma niyenda kuti nikamuchoseko mutulo." ¹² Bopunzhira bake bana kamba kuli Iye, "Mbuye, ngati agona mutulo, muzamuusha." ¹³ koma Yesu anakambapo pali iyi infa, koma anaganizila kuti akamba pakugona kopumula. ¹⁴ koma Yesu anabauza potuba, "Lazaro afa. ¹⁵ Ndipo ndine okondwela, kamba kaimwe, kuti sininalipo pakuti mukakulupilile. Tiyeni tiyende kwamene alili." ¹⁶ Thomasi anali kuitanidwa Didimasi, anakamba kuophunzira anzake, "Tiyeni naise tikafe ndi Yesu." ¹⁷ Pamene Yesu anabwela, anapeza kuti Lazaro anaikidwa mu manda anankalamo ndi masiku anai. ¹⁸ Koma Betaniya inali pafupi ndi yerusalemu, panali muyeselo kumi ndi asanu katalamukila. ¹⁹ Ayuda ambiri anabwela kuli Mariya ndi Malita, anabwela kuatontoza paza mubale wao. ²⁰ koma Malita, pamene anamvela kuti Yesu alikubwela, anaenda kuka mukumanya, koma Mariya analinkhezi mu nyumba. ²¹ Marita ananena kuli Yesu, "Mbuye, asembe mwenzepo, mubale wanga sembe sianafe. ²² Angankhale manje, niziba kuti chilichonse chamene ungapempe kwa Mulungu, azakupasa." ²³ Yesu anamuyanka kuti, mubale wako azaukafuti." ²⁴ Marita ananena ndi iye, "Niziba kuti azauka nso pakuuka kosirizira." ²⁵ Yesu ananena kuli iye, "Ndine kuuka ndiponso ndine umoyo; iye wamene akulupilila muli ine, angankale kuti afe, azankala ndi moyo; ²⁶ Ndiponso alionse alina moyo ndi kukulupilila ine sizafa. kodi ukulupilila ichi?" ²⁷ Ananena ndi iye, "Inde, Ambuye, nikulupilila kuti ndi mwe krithu, mwana wa Mulungu, wamene alikubwela muno muziko." ²⁸ pamene anakamba izi, anaenda kuitana mubale wake Mariya pambali, ndi kunena, "kuti aphunzisi akuitana iwe." ²⁹ pamene anamvela izi anaenda kamusana kuli iye. ³⁰ Koma Yesu siana bwele pamene apo mumuzinda koma anali kumalo ena kwamene Marita anamukumanya. ³¹ Ndi iwo ayuda, amene anali ndi emve mu nyumba anali kumutontoza, anaona Maria kunyamuka kwamusanga kuchoka panja, ndi kumukonka, ndi kuganizila kuti analikuyenda ku manda kuyenda kulila. ³² Ndiponso Mariya pamene anafika pamene Yesu anali ndi kumuona, anagwela pamapazi yake nikunena kuti, "Mbuye, asembe mwenze pano, mubale wanga sembe sianafe." ³³ Pamene Yesu anamuona kulila, ndi ayuda ameneana bwela kuli iye ndi iwonso analikulila, chinamukata kumutima ndi kumuvuta; ³⁴ Ananena, "kuti mwamu goneka kuti?" Anakamba kuli iye, "Ambuye, bwelani muone." ³⁵ Yesu analila. ³⁶ Koma ayuda anane, "Onani mwamene anali kumukondela Lazaro!" ³⁷ koma benabake ananena, kodi ngati uyu munthu anaseguliwa menso aleka bwanji kuti uyu munthu afe?" ³⁸ Ndiponso Yesu, popezeka okumudwisiwa mwa iye eka, anaenda ku manda. koma kunali chimugodi, ndiponso kuna fakiwa mwala. ³⁹ Yesu ananena, "chosaniko mwala." Marita, mubale wa Lazaro, wamene anafa, ananena kuli Yesu, "Mbuye, zino ntawi natupi yayamba kuola, ankala okufa masiku anai." ⁴⁰ Yesu ananena kuli iye, "kodi sininakambe kuli iwe kuti, Ngati mwakulupilila muzaona ulemelelo wa mulungu?" ⁴¹ Koma anachosako mwala. Yesu ananyamula menso yake ndi kunene kuti, "Atate, nikuyamikani popezakuti mumani mvela ine. ⁴² Ninaziba kuti mumani mvela lyonse, koma ni chifukwa chagulu yamene yaimilila ndikuzinguluka ndi kukamba kuti ninanena izi, pakuti akulupilile kuti munanituma." ⁴³ Pochoka kukamba izi, analila ni liwu lapamwamba, "Lazaro, choka!" ⁴⁴ Ndi munthu okufa anachoka; mapazi yake ndi manja zinali zomangidwa na nyula, ndi pamanso pake panamangiwa na nyula. Yesu ananena kuli bemve, "Mumangusuleni na kumusiya aende." ⁴⁵ Ndiponso ayuda ambiri amene anabwele kuona Mariya ndi zamene Yesu anachita, Ana mukulupilila; ⁴⁶ koma benangu bana enda kuona afarisi ndiponso anabauza zinthu zamane Yesu anachita. ⁴⁷ Ndiponso akulu ansembe ndi afarisi anaita kabungwe pamodzi ndi kunena, "kodi tingachite bwanji? Uyu muntu achita zodabwisa zambiri, ⁴⁸ Ngati tamusiilila chabe eka, onse azakulupilila muli iye; Aroma azabwela pamodzi ndi kutenga malo yatu ndi zikolatu." ⁴⁹ Koma umoji palibemve, kefasi, wamene anali mukulu wansembe chija chaka, ananena kulibemve "Simuziba chilichonse. ⁵⁰ simuganiza kuti ni chabwino munthu umodzi kufela banthu bonse pakuti ziko lonse lisaonongeke." ⁵¹ Koma ichi, sianakambe kuchokela kwa iye eka. koma, kunkala mukulu wa nsembe chaka chija, Anapeleka uneneli kuti Yesu azafela ziko; ⁵² osati zikochabe leka, Ndiponso kuti bana onse a Mulungu amene

anasalangana akabwerere pamodzi mu umozi. ⁵³ pakuti kuchokela lamene lija siku banapangana mwamene anga mupayile Yesu. ⁵⁴ Kuchokela apo Yesu sianaendelepo potuba ku Ayuda, koma anaenda kuchokakuja muziko inali pafupi na chipululu mumuzinda oitanidwa Efuremu. Kuja anankala ndi ophunzila bake. ⁵⁵ Koma pasakha ya Ayuda, inali pafupi, Ndiponso ambiri anaenda mu yerusalemu kuchoka mu ziko bakalibe kuenda ku pasakha kuti akaziyelese iwo oka. ⁵⁶ Analikusakila Yesu, ndi kukambisana iwo oka pamene anaimilila mutempele," kodi munganiza chani? Kuti sizabwela ku phwando?" ⁵⁷ Koma mukulu wa nsembe ndi afarisi anapasa ndandanda kuti ngati alionse anaziba kwamene Yesu anali, afunika akambe pakuti amugwire iye.

Chapter 12

¹ Masiku asanu na imozi pamene pasaka sinafike, Yesu anabwela ku Betani, kwamene Lazalo analili, wamene Yesu anaukisa ku bakufa. ² Kwamene kuja banamu konzela chakudya cha usiku, Malita anali kugabanisa chakudya, koma Lazalo anali pamozi nabaja bamene banankala pa malo yodyelapo pamozi na Yesu. ³ Chinakonkapo kuti Maria anatenga ka gubu ka mafuta onunkila yopangiwa na Nalidi yotuba ya mutengo wapatali, naku zoleka mendo ya Yesu, naku yapuputa mendo na sisi zake. Nyumba yonse inazula na kununkila kwa yaja mafuta. ⁴ Yudas Iskarioti, umozi mwa bopunzila wa Yesu, wamene anamugulisa Yesu, anakamba kuti, ⁵ "Nanga nichani aya mafuta siyanagulisiwe ndalama zokwanila fili hundredi denarii naku pasa bosauka?" ⁶ Koma ichi anakamba eve, osati chifukwa asamalira bosauka, koma chifukwa anali kawalala. Ndiye wamene anali na kasaka kosungilamo ndalama ndiponso anali kuba ndalama zamene zinali kuikiwamo muja. ⁷ Yesu anakamba kuti, "Mulekeni asunge vamene ali navo kufikila siku yoni ika mumanda ine." ⁸ Bosauka muzankala nabo ntawi zonse pakati panu. Koma ine simuzankala naine ntawi zonse." ⁹ Manje gulu ya ba Yudainaziba kuti Yesu analiko kumalo kuja, ndipo bana bwela, osati kukonka Yesu, koma kuona Lazalo, wamene Yesu anaukisa ku bakufa. ¹⁰ Bakulu ba nsembe banapangana kuti bamupaye Lazalo; ¹¹ chifukwa chake nichakuti kamba ka eve bambili banachokako naku kulupilila mu Yesu. ¹² Pa siku yokonkapo gulu ikulu inabwela ku pwando. Pamene bana mvela kuti Yesu azabwela ku Yelusalema, ¹³ banatenga matambi ya mitengo ya Palm naku yenda kukumana naye na ku punda kuti, "Hosanna!" Odala ni muntu wamene abwela mu zina ya Ambuye, mfumu ya Isirayeli. ¹⁴ "Yesu anapeza ka Kavalo kaka ngono naku ka kwelapo; monga mwamene chinalembelewa kuti, ¹⁵ "Osayopa, mwana wa Ziyoni; ona, Mfumu yako ibwela, yankala pa chonkalapo chapa Kavalo." ¹⁶ Koma bopunzila bake sibनाविम्वेसे ivi poyamba; koma pamene Yesu anakwezekewa, banakumbukila kuti ivi vintu vinalembelewa kukamba pali eve ndiponso bana chita ivi vintu kumuchitila eve. ¹⁷ Manje gulu yonse inapeleka umboni kuti banali naye pamene anaitana Lazalo kuchoka mumanda naku mu-ukisa kubakufa. ¹⁸ Nichifukwa cha ichi chamene gulu ina enda kumukumana eve, chifukwa banamvela kuti anachita chamene ichi. ¹⁹ Beve ba Falisi banakamba pakati pabo kuti, "Onani, kulibe chamene mungachite; onani, ziko yonse ya enda kumukonka eve." ²⁰ Manje benangu ba chi Giliki banalipo pa gulu ya baja banali ku yenda ku pembeza ku pwando. ²¹ Aba bana enda kuli Filipino, wamene anachokela ku Betisaida malo ya Galili, naku mufunsa, kuti, "bambo, tifuna kuona Yesu." ²² Filipino ana enda ku- uza Andulu; Andulu ana enda na Filipino, naku mu uza Yesu. ²³ Yesu ana bayanka beve nakukamba kuti, "Ntawi yafika kuti Mwana wa Muntu akwezewe. ²⁴ Zo-ona, zo-ona, niku-uzani imwe, ngati mbeu ya tiligu sinagwele mu ntaka nakufa, izankala yeka; koma ngati yafa, iza bala zipaso zambili. ²⁵ Eve wamene akonda umoyo wake azautaya; koma uja wamene auzonda moyo wake mu ziko ino azausungila umoyo wamene si usila. ²⁶ Ngati muntu aliyense ani sebenzela, mulekeni anikonke; na kwamene nilili, na eve nikwamene azankala wanchito wanga. Ngati muntu aliyense anisebenzela, Atate bazamu kwezeka. ²⁷ Manje umoyo wanga wavutika nanga nizakamba chani ine? 'Atate, nipulumuseni kunichosa kuntawi iyi?' 'Iyayi nichifukwa cha ivi chamene nabwelela muntawi iyi. ²⁸ Atate, lemekezani zina yanu.' Mau yanachoka ku mwamba kukamba kuti, "Na ilemekeza komanso nizailimekeza nafuti." ²⁹ Pamene apo gulu yamene inaimilila pamozi na eve inamvela mau inamvela monga kuna gwedezeka. Benangu banakamba kuti, "Mungeli ndiye akamukambisa." ³⁰ Yesu anakamba kuti, "Iyi liu si inakambe chifukwa changa ine, koma imwe. ³¹ Manje ni ntawi yachiweluzo cha ziko: Manje eve olamulila ziko ino azataiwa panja. ³² Pamene ine nikwezewa kuchoka pa ziko yapansi, niza donsa bonse kuli ine." ³³ Ichi anakamba ku langiza njila ya imfa yamene eve aza mwalilila. ³⁴ Gulu ina muyanka eve, "Tinamvela mu lamulo kuti Kristu azankala na umoyo osasila. Manje iwe ungakambe bwanji kuti, 'Mwana wa Muntu ayenela ku imisiwa mumwamba?' Nanga wamene uyu Mwana wa muntu nindani?" ³⁵ Yesu anayanka kuti, "Ku unika kuzankala na imwe kwa ka ntawi ka kangono. Endani pamene mukali na ku unika, mwakuti mfizi isaku pitilileni. Eve wamene aenda mu m'mfizi saziba kwamene aenda. ³⁶ Pamene mukali na ku unika, kululupilani mu ku unika mwakuti munkale bana baku unika." Yesu anakamba ivi vintu naku chokapo kuyenda kubisama. ³⁷ Ngankale kuti Yesu anachita volangiza vambili pamaso pabo, koma sibana kululupile muli eve ³⁸ kufikiliza mau ya muneneli Yesaya, yamene anakamba kuti: "Ambuye, nanga nindani wamene anakululupila mau yatu, komanso nikuli uti kwamene kwanja ya Ambuye ina oneseva?" ³⁹ Nichifukwa cha chamene ichi sibana kululupile, chifukwa Yesaya anakamba futi kuti, ⁴⁰ "Anaba vala pamenso pabo, ndipo anaba kosesa mitima zabo; ndaba asembe banakwanisa kuona na menso yabo naku mvesesa na mitima zabo, naku tembenuka, ndipo asembe ninaba polesa. ⁴¹ Yesaya anakamba ivi vintu chifukwa anaona ulemelelo wa Yesu na kukamba pali eve. ⁴² Koma ngankale kuti vinali njila iyi, bambili basogoleri banakulupilila muli Yesu; koma chifukwa cha Afalisi, sibanalil kuvomela kuyopa kuti bangaba pishe mu Synagogo. ⁴³ Bana konda matamando yochoka kuli bantu kuchila matamando yochokela kuli Mulungu. ⁴⁴ Yesu anapunda naku kamba kuti, "Wamene akulupilila muli ine, akulupilila osati muli ine chabe koma na muli

wamene anani tuma ine,⁴⁵ ndiponso wamene aona ine aona wamene ananituma.⁴⁶ Ine ninabwela ngati nyali mu ziko, mwakuti eve wamene akulupilila muli ine asasale mu m'mfizi.⁴⁷ Ngati aliyense amvela maaui yanga koma saya sunga, Sinimuweluza; chifukwa ine sininabwelele kuweluza ziko, koma kuipulumusa.⁴⁸ Eve wamene akana ine na uja wamene salandila mau yanga, ali naye wamene amu weluza. Mau yamene nakamba yazamu weluza pa siku yosiliza.⁴⁹ Chifukwa ine sinina kambe vanga paneka, koma ni Atate bamene banani tuma, bamene banani pasa lamulo ya vumene niyenela kukamba na vokambapo.⁵⁰ Niziba kuti lamulo yake ni moyo wamene susila, ichi nichamene nikamba-monga mwamene Atate banakambila kuli ine, nimwamene nikambil."

Chapter 13

¹ Manje pamene ikalibe kufika Phwando ya Pasaka pamene Yesu anaziba kuti nthawi yake yakwana kucoka kuno kudziko kuyenda kwa Atate -mwamene anabakondela bake amene anali muziko -anabakonda kufikila kulasti. ² Manje satana enze anaika kudala m'mtima wa Yudasu iskarioni mwana mwamuna wa Simoni, kuti apacike Yesu ³ Anaziba kuti ba Tate anamupasa zonse kwayeve mumanja mwake ndipo kuti anacokela kwa Mulungu ndiponso enzobwelela kwa Mulungu. ⁴ Ananyamuka penzo dyela ndipo anavula vovala vake vakunja. Pamene apo anatenga tawelo noimanga mumsana. ⁵ Pameneapo anatila manzi mu dishi noyamba kusambika mendo ya ophunzira nobapukuta na tawelo yamene enze anamanga mu msana mwake. ⁶ Anabwela kwa Simoni Petulo, ndipo Peturo anakamba ati kwa yeve, "Ambuye, nishi muzasambika mendo yanga?" ⁷ Yesu anamuyankha nokamba ati, "camene nicita suvesesa manje, koma uzavesesa pasogolo." ⁸ Petulo anakamba ati kwa eve, "Suzasambikako mendo yanga." Yesu anamuyankha ati, "Ngati sinizakusambika iwe, ulibe mbali naine." ⁹ Simoni Petulo anamuza kuti, "Ambuye, musasambika mendo yanga cabe, komaso manja yanga ndi mutu wanga" ¹⁰ Yesu anamuza ati, Yeve wamene wasambikiwa alibe cofuna, koma cabe kusambika mendo yake, koma nibotubilatu, ndiwe otuba, koma sibonse." ¹¹ (Cifukwa Yesu anaziba wamene azamupacika; nicifukwa cake anakamba ati, sibonse botuba.") ¹² Ndipo pamene Yesu anabasambika mendo notenga vovala vake nonkhala pansu futi, nobwela ukamba ati kulibeve, bushe muziba wamene nakucitilani? ¹³ Muniitana kuti 'm'mphunzisi' ndi 'Ambuye' ndipo mukamba bwino, cifukwa ndiye mwamene nilili. ¹⁴ Manje ngati ine, Mbuye ndi M'mphunzisi, nasambika mendo yangu, mufunika naimwe kusambikana mendo mweka-mweka. ¹⁵ Cifukwa cakuti nakupasana cokopelako kuti mucite mwamene nacicita kwa imwe ¹⁶ Nikamba zooni, nikamba kwa imwe, wanchito sapambana bosu wake; kapena otumikila kupambana wamene amutuma. ¹⁷ Ngati muziba ivi vinthu, ndimwe odalisika ngati muvici. ¹⁸ Sinikamba za imwe monse; niziba baja bamene ninasankha -koma ciliso kuti mau ya Mulungu yakwanilisike: 'yeve wamene akudya buledi yanga kanyamulidwa katende kake kasushana naine.' ¹⁹ Nikuuzani izi manje vikalibe kucitika kuti vikacitika, mungakhulupile kuti NDINE INE. ²⁰ Kukamba zooni, nikamba kuli imwe, yeve wamene alandila wamene natuma, alandila ine, ndipo yeve wamene walandila ine, alandila wamene ananituma ine." ²¹ Pamene Yesu anakamba izi, anavutika m'mzimu, anaperekela umboni nokamba ati, "Nikuuzana coonadi, nikamba kuli imwe kuti umozi waimwe azanipacika." ²² Ophunzila banayanganana, kudabwa-dabwa kuti nindani wenzu kambapo. ²³ Umozi wa bomphunzila wake, wamene Yesu anakonda, analigone pa tebo kusamila pa pacifuwa ca Yesu. ²⁴ Simoni Peturo pameneapo anaceula kuli ophunzira uyo nokamba ati, "Tiuze wamene akambapo." ²⁵ Pamene apo anasamila pa chifuwa pa Yesu nokamba kuliyeye ati, "Ambuye nindani?" ²⁶ Pamene apo Yesu anayankha ati, "niwuyo wamene nizasunsa ka bledi nopasa yeve." So pamene anasunsa ka buledi, anapasa Yudasu mwana mwamuna wa Simoni Iskarioni. ²⁷ Manje, pambuyo pa buledi, satana anangena mwa yeve, ndipo Yesu anakamba nayeve ati, "Pavamene ucita, cita mwamusanga." ²⁸ Manje kulibe wamene anali gone pa tebo wamene anaziba cifuka camene anakambila so kwa yeve. ²⁹ Benangu anaganiza kuti, cifukwa cakuti Judasi enzeli na chola ca ndalama, Yesu anakamba nayeve, Gula wamene vifukika pa phwando," kapene apaseko vinangu kuli bosauka. ³⁰ Pamene Yudasu alandila buledi, anabwela acokapo pamene apo. Kwenzeli usiku. ³¹ Pamene Yudasu anayenda, Yesu anakamba ati, "Manje mwana Mwamuna wa Munthu walemekezeka, ndipo Mulungu walemekezeka mwa yeve. ³² Mulungu azamulemekeza yeve mwa yeve yeka, ndipo azamulemekeza yeve pamene apo. ³³ Bana bang'ono, nili na imwe pakanthawi ka ng'ono. Muzanisakila, ndipo mwamene ninakambila kuli baYuda, 'Kwamene niyenda, simungabweleko.' Manje nikamba cimozi -mozi kwa imwe. ³⁴ Nikupasani lamulo ya manje, kuti mukondane wina ndi mzake; monga mwamene nakukondelani, cimozi-mozi mukondane wina ndi mzake. ³⁵ Mwaici aliyense azaziba kuti ndimwe uphunzila banga, ngati mulinaco cikondi cawina na mzake." ³⁶ Simoni Petro anakamba kwa yeve ati, "Ambuye, muyenda kuti?" Yesu anayankha ati, "Kwamene niyenda, sunganikonkhe manje, koma uzanikonkha pambuyo pake" ³⁷ Petro anakamba kwayeve ati, "Ambuye, cifukwa nicani siningakonkhe manje? Nizapasa moyo wanga cifukwa caimwe." ³⁸ Yesu anayankha ati, "Kansi ungapase moyo wako cifukwa caine? Nikamba zoonadi, nikamba kwa iwe, tambala akalibe kulila uzanikana ine katatu."

Chapter 14

¹ "Musaleke mitima yanu ivutike. Khulupirilani mwa Mulungu, ndipo khulupirilani mwainenso. ² Munyumba ya Tate wanga alimo malo yonkalamo yambiri. ngati sichinali so, sembe ninakuuzana, chifukwa nayenda kukonza malo anu imwe. ³ Nikaenda no kukonzhelani malo imwe, nizabwela ndipo nizakulandilani kwaine pakuti kwamene nili naimwe mukhankaleko. ⁴ Muiziba njila ya kwamene niyenda." ⁵ Thomasi ananena kwa Yesu, "Ambuye, sitiziba kwamene muyenda, nanga njila tingaiziba bwanji?" ⁶ Yesu anamuza ati, ine "ndine njila, ndine choonadi ndipo ndine moyo, kulibe wina angabwele kwa Tate kupanda mwaine. ⁷ Ngati mwenze kuniziba asembe munamuziba naeve Tate wanga. Kuchoka apa mwamuziba, ndipo mwamuona." ⁸ Filipo anakamba kwa Yesu, Ambuye, tilangizeni Atate, icho chabe chizatikwanila." ⁹ Yesu anakamba kwa iye, "nankala naimwe ntawi itali maninga koma sumuniziba, Filipo? Aliense aniona amuona Tate. Manje iwe ungakambe bwanji ati, 'tilangize Tate'? ¹⁰ Ninshi sukhulupirila kuti ine nili muli Tate na Tate ali mwaine? Mau yamene nikuuzani imwe sinikamba mu mphavu zanga iyayi, koma ni Tate wamene ankhal mwaine wamene achita chinto yake. ¹¹ Nikhulupirileni kuti ine nili mwa Tate, na Tate ali mwaine, ndiponso khulupirani chamachitidwe yamene. ¹² Choonadi, Choonadi, nikuuzani kuti uyo wamene akhulupirila mwaine azachita nchito zamene nichita, ndipo azachitanso nchito zikulu kupambana nazamene izi chifukwa ine niyenda kwa Tate. ¹³ Zonse zamene muzapempa muzina langa, nizakuchitilani pakuti Tate alemekezediwe mu Mwana mwamuna. ¹⁴ Mukanipempa chilichonse muzina yanga, nizakuchitilani. ¹⁵ Ngati munikonda imwe, muzasungu malamulo yanga. ¹⁶ Ndipo nizakupempelelani kwa Tate wanga, naye azakupasana Omipuzya(Omitontoza) wina pakuti akankhale naimwe masiku onse: ¹⁷ Muzimu wa choonadi. Wamene ziko singalandile chifukwa sinamuonepo ndipo simuziba iyayi. Koma inu mumuziba, chifukwa ankhal naimwe ndipo anzankhal mukati kaimwe. ¹⁸ Sinizakusiyani mweka; nizabwela futi kwainu. ¹⁹ Ndipo ntawi ing'ono ziko sizanionanso, koma imwe muniona. Chifukwa ine nili na umoyo, nainu muzankala na umoyo. ²⁰ Pasiku ija muzaziba kuti ine nili mwa Tate, ndipo inu muli mwaine, naine nili mwainu. ²¹ Wamene ali namalamula yanga ndipo ayasunga ninsi niwamene anikonda, elyo wamene anikonda azakondewa na Tate wanga, nainenso nizamukonda na kuilangiza ine kwaeve. ²² Yuda (uyu si Isikario iyayi) anuza Yesu ati, "Ambuye, nanga nichani muzazilangizi mweka kwaise osati ku ziko?" ²³ Yesu anamuyanka no kamba kwaeve kuti, "ngati muntu aliynse anikonda, azasunga mau yanga. Tate wanga azamukonda, ndipo tizabwela kwaiye nakumanga nyumba yatu naye. ²⁴ Wamene sanikonda samasunga mau yanga. Mau yamene munvela siyachokela kwaine koma niyochokela kwa Tate wamene ananituma. ²⁵ Nakuuzani zinthu izii, nikali kunkhal naimwe. ²⁶ Koma, Mutonthozi - Muzimu Oyela wamene Tate azatuma muzina langa - iye azakupunzisani zonse ndipo azakukumbusani zonse zamene nakuuzani ine. ²⁷ Nakusiyilani mutendere; nakupasani mutendere. Sinikupasani mwamene ziko ipasila. Mutima wanu usavutike, ndipo musayope. ²⁸ Munanvela kuti nakuuzani imwe, 'Ine niyenda, ndipo nizabwelanso kwaimwe.' Ngati mwenzonikonda, asembe mwakondwera kuti niyenda kwa Tate, chifukwa Tate nimukulu kunichila ine. ²⁹ Manje nakuuzani chikalibe kuchitika, chikachitika muzakulupirila. ³⁰ Sinizakambanso futi zambiri na imwe, chifukwa olamulila ziko ili lapansi abwela. Alibe mphavu pa ine, ³¹ koma pakuti ziko izibe kuti ine nikonda Tate, nichita chabe mwamene Tate ananilamurila. Tiyeni tinyemuke, tichokepo apa. ³⁰ Sinizakamba vambili manje na imwe, chifukwa eve oweluzo ziko ino abwela. Eve alibe mpavu pali ine, ³¹ koma kuti ziko izibe kuti ine nikonda Atate, nichita monga mwame Atate banani uzila. Tiyeni ti ime tichokepo pano."

Chapter 15

¹ Ine ndine mpesa weni-weni, Atate wanga ndiye mlimi wa dimba. ² Iye amajuwa msambo uliwonse mwaine wamene siubala viphaso, koma amajuwilila msambo uliwonse wamene ubala viphaso, kuti ubale viphaso vyambiri. ³ Inu ndinu woyela kale chifukwa ca mau amene nalankhula namwe. ⁴ Nkalililani mwaine, naine mwa inu. Monga msambo suungabale viphaso pa weka pokapo ngati wankhala ku chimutengo ca mpesa, pokapo munkhalilile mwaine. ⁵ Ine ndine mpesa, inu ndinu msambo wanga. Yense amene ankhala mwaine na ine mwa iye, azabala viphaso zambiri; popanda ine simukacite kanthu. ⁶ Ngati aliwonse sankhalilila mwaine, ataidwa ngani msambo na kuyuma, Misambo yatele imatengedwa ndikuyiponya ku moto kuti ipye. ⁷ Ngati muzankhalilila mwaine, na mau anga muli imwe, Pemphani ciliconse camene mufuna, cizacitidwa kwa inu. ⁸ Atate anga amalemekezedwa muli izi, kuti mubale viphaso zambiri ndipo muzionese kuti ndinu wophunzila wanga. ⁹ Monga atate andikondela, nainenso ndikukondani. Nkhalililani mu Chikondi canga. ¹⁰ Ngati musunga malamulo anga, muzankhalilila muchikondi canga, monga ine nisunga malamulo ya Atate nonkhalilila mu Chikondi cake. ¹¹ Nalankhula namwe izi kuli imwe kuti chimwemwe canga cikale mwainu, ndipo kuti chimwemwe cikwanile. ¹² Lamulo langa ndi iyi, kuti mukondane wina ndi muzace, monga mwamene ine ndikukondelani inu. ¹³ Palibe amene alindi chikondi copambana ici, kuti anataya moyo wake chifukwa ca azake. ¹⁴ Ndinu anzanga tsopano ngati muchita zimene ndikulamulilani. ¹⁵ Sindizakuyitanani inu anchito, chifukwa wanchito saziba zimene mbuye wake acita. Ndikuitanani inu anzanga, chifukwa zonse zimene ndinamvwa kuchokela kwa Atate, nakuziwisani. ¹⁶ Inu simunandisankhe ine, koma ndinakusankhani, nosakiwa kuti mupite mukabale viphaso ndipo viphaso vinkalilile. Ndipo Atate azakupasani ciliconse cimene muzapempha muzina langa azakupasani. ¹⁷ Izi zimene nikulamulilani kuti mukondane wina ndi muzace. ¹⁸ Ngati dziko lapansi ikuzondani, zibani kuti inayamba kuzonda ine, ikalimbe kukuzondani inu. ¹⁹ M'kanankhala anthu a dziko lapansi, likana kukondani ngati anthu ake. Koma chifukwa simulibadziko lapansi ndipo chifukwa ndinakuitanani kukucosani mudziko, nchifukwa cake dziko ikuzondani. ²⁰ Kumbukilani mau amene ndinalankhula nanu kuti, palibe wanchito amene apambana bwana wake. Ngati bananisausa ine, bazakusausani naimwe; Ngati anasunga mau anga azasunganso yanu. ²¹ Azacita zonse izi kwainu chifukwa ca ine, samuziba wamene ananituma ine. ²² Kutu ine sindinabwele nakukamba nawo, sembe balibe kucimwa, koma manje balibe cokanila mlandu wawo. ²³ Amene azonda ine azondanso Atate anga. ²⁴ Ine kuti ndiliba cite nchinto iliconse pakati pawo zinthu zimene wina sanacitepo iwo sakanakala wocimwa. Manje chifukwa aona zodabwisa izi, ndipo andizonda ine pamodzi ndi Atate anga. ²⁵ Koma zacitika telo kuti zikwanilise zimene malembo analembedwa mumalamulo; "Ananizonda ine popanda chifukwa." ²⁶ Pamene muthontozi - wamene ndizathuma kucokela kwatate, amane ali Mzimu wa coonadi, wocokela kwa Atate - azacitila umboni za ine. ²⁷ Inu municitila umboni, chifukwa mwankhala naine kucokela poyamba.

Chapter 16

¹ Nakamba ivi vintu kuli imwe kuti musataike. ² Bazakupilikisani muma Sinagogo. Koma ntawi izabwela yamene aliyense wamene azapaya imwe azaganizila kuti asebenzela Mulungu. ³ Bazachita ivi vintu chifukwa sibana baziye Batate olo Ine. ⁴ Nakamba ivi vintu kuli imwe mwakuti ngati ntawi yabo yafika, muzakakumbuka kuti ninaku-uzani pa va bemve. Sininaku-uzeni pali ivi vintu poyamba, chifukwa Ninali nikali naimwe. ⁵ Koma apa ma je Noiyeenda kuli wamene ananituma, koma kulibe aliyense pali imwe wamene anifunsa, 'Nanga muyenda kuti?' ⁶ Koma chifukwa nakamba ivi vintu kuli imwe, chifundo chazuka mu mitima zanu. ⁷ Koma chazoonu niku-uzani imwe, nichabwino kuti ine niyende. Chifukwa ngati ine sinizaenda, eve Otontoza sazabwela kuli imwe, koma ngati ine naenda, nizamutuma kuli imwe. ⁸ Pamene azabwela, eve Otontoza azalangiza ziko kuti niyolakwa pa za chimo, paza chilungamo, komanso napali chiweluzo - ⁹ pa chimo, chifukwa sibakulupilira muli Ine; ¹⁰ pali za chilungamo, chifukwa Ine niyenda kuli Batate, ndipo simuzayamba kuniona; ¹¹ komanso pali chiweluzo, chifukwa eve olamulila ziko anaweluziwa. ¹² Nikali navambili vamene nifuna kukamba naimwe, koma simungavimvesese apa manje. ¹³ Koma pamene eve, Muzimu wa Chazo-ona, azabwela, azaku sogolelani muvazo-ona vonse, chifukwa eve sazakamba vake eka. Koma azakamba vonse vamene azamvela, ndipo azaku-uzani vintu vamene vamene vizabwela. ¹⁴ Azapeleka ulemelelo kuli ine, chifukwa azatenga kuchosa pali vanga nakuku-uzani imwe. ¹⁵ Vonse vamene Batate balinavo nivanga. Chifukwa cha ichi, nakamba kuti Eve Muzimu azatenga kuchosa pali vanga nakuku-uzani imwe. ¹⁶ Kwa ntawi ing'ono imwe simuzaniona nafuti, ndipo pakapita kantawi kang'ono muzaniona. ¹⁷ Manje bena pabopunzila bake banakamba wina na muzake kuti, "Nanga ichi chamene atiuza ise kuti, 'Kantawi kang'ono imwe simuzaniona futi koma futi kantawi kang'ono muzaniona,' futi, 'chifukwa ine nienda kuli Batate?'" ¹⁸ Mwa ichi banakamba kuti, "Nanga ichi nichani chamene akamba kuti, 'Kwa ka ntawi kang'ono?' Ise sitiziba vamene akambapo." ¹⁹ Yesu anaona kuti banali kufuna kumufunsa, ndipo anabauza kuti, "Nanga ichi ndiye chamene muzifunsa pamweka, chamene nitantauza pakukamba kuti, 'Kwa ka ntawi kang'ono koma simuzaniona nafuti, ndipo mwa ka ntawi kang'ono koma muzaniona?'" ²⁰ Chazo-ona, chazo-ona, niku-uzani imwe, muzakalila momvesa chifundo, koma ziko izakakondwela. Muzankala bozula na chifundo, koma chifundo chanu chizasandulisiwa kunkala chimwele. ²¹ Pamene muzimai abala amamvesa chifundo chifukwa ntawi yake yafika, koma akabala mwana, samakumbukila vomvela kubaba chifukwa chakuti muntu abadwa paziko. ²² Onani apa mu mvesa chifundo manje, koma nizakuonani nafuti, ndipo mitima zanu zizakondwela, ndipo kulibe aliyense wamene azakwanisa kuchosa chimwemwe mumitima zanu. ²³ Pasiku ija simuzakanipempa ine kantu kali konse. Zo-ona, zo-ona, nikamba kwa imwe, ngati muzapempa chintu chilichonse kuli Batate muzina yanga, bazakupasani imwe. ²⁴ Kufikila apa kulibe chamene imwe mwapempa muzina yanga. Pempani ndipo muzapasiwa, mwakuti chimwemwe chanu chinkale chofikilisiwa. ²⁵ "Nakamba ivi vintu kuuza imwe kupitila muma pinda, koma ntawi izafika yamene nizaleka kukamka naimwe muma pinda, koma nizaku-uzani po-onekela paza Batate. ²⁶ Pasiku ija imwe muzapempa muzina yanga koma sinikamba kuti nizakupempelani imwe kuli Batate, ²⁷ chifukwa Batate beve bakukondani imwe chifukwa imwe munanikonda ine ndiponso chifukwa chakuti manakulupilila kuti ine ninachokela kuli Batate. ²⁸ Ninachokela kuli Batate, ndipo ninabwela muziko. Futu, nizasiya ziko naku enda kuli Batate. ²⁹ Bopunzila bake banakamba kuti, "Onani, apa manje mwakamba momvekesesa mosasebenzesa mapinda. ³⁰ Manje tiziba kuti imwe muziba vintu vonse, ndipo simufunika kuti muntu aliyense afunse ma funso. Chifukwa cha ichi, tikulupilila kuti imwe munachokela kuli Mulungu." ³¹ Yesu anabayanka nati, "Nanga mwakulupilila manje?" ³² Onani, ntawi izabwela, zo-ona, koma futu yafika, pamene imwe muzapatuliwa, aliyense kunyumba kwake, ndipo imwe muzanisiya neka. Koma sinili neka chifukwa Batate bali naine. ³³ Nakamba ivi vintu ku-uzani imwe mwakuti mwa ine munkale na mutendere. Muziko muzankala na vovutisa, koma nkalani bolimba mutima, Nagonjesa ziko."

Chapter 17

¹ Pamene Yesu anasiliza kukamba ivi, ananyamula menso yake kumwamba nakukamba; Atate, nthawi yafika, lemekezani mwana wanu kuti mwana wanu akulemekezeni. ² Mwamene munamupasila ulamuliro pa munthu ali wonse pakuti akapase umoyo osata kuli bonse bamene anapasiwa. ³ Uyu nimoyo osata; kuti bamizibeni, mulungu eka wachonadi, ndipo wamene otumiwa Yesu Kristu. ⁴ Ninamulemekezani pa ziko. Ninasiliza nchito yamene munanipasa kucita. ⁵ Manje, atate, nilemekezeni pamodzi nainu na ulemelelo wamene ninali nawo pamene ziko ikalibe kupangiwa. ⁶ Ninaionesa dzina lanu ku anthu amene munanipasa kuchokela mu dziko. Banali anthu anu, ndipo munanipasa, ndiponso banasunga mau wanu. ⁷ Apa baziba ati vonse vamene munanipasa vinachokela kuli inu, ⁸ ndiponso ninabapasa mau wonse munanipasa. Banalandila nakuziba banaziba ati ninachokela kuli inu, ndiponso bana khululupilira kuti munanituma. ⁹ Nibapempelela, sinipempelela ziko koma baja bamene munanipasa. ¹⁰ Vonse vanga nivanu, navanu nivanga, ndiponso nilemekezedwa muli iwo. ¹¹ Sinili muziko, koma aba bantu bali muziko ndiponso nibwela kwainu. Atate oyela, basungeni muzina lanu munanipasa kuti bankale umodzi, monga ise tili umodzi. ¹² Pamene ninali nabo, ninabasunga muzina lanu, lamene munanipasa. Nina bacingiliza, kulibe aliyose anaonongeka, kuchoselako chabe mwana wa chitayiko, kuti lembo likwanisidwe. ¹³ Apa nibwela kwainu koma nikamba izi zinthu muziko pakuti bankale nachmwemwe chosililila mulibeve. ¹⁴ Ninabapasa mau yanu, ndipo ziko yaba zonda cifukwa sibamu ziko, monga ine sinili wamu ziko. ¹⁵ Sinimpempa kuti mubachose muziko, koma mubasunge kuchokela kumudani. ¹⁶ Siba muziko monga ine sindine wamu ziko. ¹⁷ Bapatululeni muchonadi, cifukwa mau yanu ni chonadi. ¹⁸ Monga mwamene munanitumila muziko, naine nabatuma muziko. ¹⁹ Cifukwa chabeve ninazi pantulula, pakuti nabeve bapatuluke muchonadi. ²⁰ Sinimpempelela chabe aba, koma nabonse abo bazakhululupira muli ine kupitila mumau yabo. ²¹ Pakuti bonse bankale umodzi, monga inu, Atate muli muli ine, ndiponso nilimuli inu. Nipempela kuti bankale muli ise pakuti chalo chika khululupire ati munani tuma. ²² Ulemelelo wamene munanipasa, ninabapasa, pakuti bankale umodzi, monga mwamene tili bamodzi. ²³ Ine muli inu, ndipo inu muli ine. Pakuti basilizike muli umodzi, pakuti ziko ikazibe ati munanituma ndiponso mubakonda monga mwamene munikondela. ²⁴ Atate, nifuna kuti bonse abo munanipasa bankale naine kwamene nilili pakuti bakaone ulemelelo, wamene mwanipasa. Cifukwa munanikonda pamene pakalibe kupangiwa kwa ziko. ²⁵ Oyela atate, ziko sinamizibeni, koma ninamizibani; ndiponso aba baziba ati munanituma. ²⁶ Ninazibisa zina lanu kulibeve, ndiponso nizazibisa pakuti chikondi chamene munanikondelako chinkale muli beve, ndipo nizankala muli beve."

Chapter 18

¹ Pamene Yesu ananena aya mau, anayenda ndi ophunzila bake kumhalo yenangu muchigwa cha Kidironi, mumunda mwamene Iye na ophunzila bake anangena. ² Koma Yudase, wamene enzofunika kumugulisa iye, naye enzo yaziba malo yaja, chifukwa kambiri Yesu analikuyenda kumhalo aja ndi ophunzila bake. ³ Koma Yudase, pamene analandila gulu ya masilikari kuchoka kubakulu bansembe ndi ku Afalise, ndiponso alonda, anabwela ndi miyuni, ndi nyali, ndi zida. ⁴ Koma Yesu, wamene analikuziba zonse zamene zenzo chitika kuli iye, anapitiliza ndi kuba funsa, "kodi musakila ndani?" ⁵ Bana muyanka iye, "Yesu waku Nazareti," Yesu anabayankha, "Ndine." Yudase, wamene anamugulisa iye, aniyimilila na asilikale. ⁶ Ndipo pamene anakamba kulibemve, "Ndine," anabwerela kumbuyo na kugwela pansi. ⁷ Ndiponso anabafunsa kuti, "Nanga ni ndani wamene musakila?" Nafuti ananena, "Yesu waku Nazareti". ⁸ Yesu anayanka, "nenze nakuuzani kuti Ndine. ngati ndine wamene musakila, siyani baja bayende." ⁹ Ichi chinali mu ndondomeko yofikiliza mau yamene enze anakamba: "pali baja bamene munanipasa, sininasobese alionse." ¹⁰ Ndiponso Simoni Petulo, wamene anali na lupanga, anaichosa ndi ku chaya wa nchito wabakulu bansembe ndikujuba kwatu kwake. Uyu wamene wa nchito enze kuyitaniwa Malikasi. ¹¹ Yesu ananena kuli Petulo, "Bwezelamo lupanga mumhalo yake. Kodi nizamwe mu kapu yamene Atate anipasa?" ¹² Koma gulu yama soja ndi mukulu wama soja na alonda Ayuda, anamugwila Yesu na kumumanga. ¹³ Banayambirila kumupeleka kwa Annasi, anali mupongozi wa Kefasi, wamene anali mukulu wansembe chaka chija. ¹⁴ Koma Kefasi analiwamene anatandizila Ayuda kuti chingawame kuti munthu umozi afele banthu. ¹⁵ Simoni Petulo anakonka Yesu, ndiwina wao ophunzila bake anachita chamene icho, koma uja ophunzila analiozibika kubakulu ba nsembe, ndiponso anangena ndi Yesu mumhalo mwa akulu ansembe; ¹⁶ koma Petulo anali imilile panja pakomo. Koma wina wa ophunzila bake, wamene anali kuzibika kubakulu bansembe, anayenda panja ndikukamba namukazi wamene anaimilila pakomo ndi kumungenesa mukati Petulo. ¹⁷ Koma wanchito mukazi, wamene anaimilila pakomo, ananena kuli Petulo, "Kodi sindiwe wa amozi ophunzila wa uyu munthu?" Anakamba, "sindine." ¹⁸ Koma anchito ndi alonda anayimilila paja, anapanga mulilo, chifukwa kunali ko zizila, ndiponso anali kuzifundisa iwo oka. Petulo anali nabeve, anayimilila nao pamene enza kuzifundisa eka. ¹⁹ Ndipo mkulu wa ansembe anafunsa Yesu pa ophunzila bake ndi chipunziso. ²⁰ Yesu anamuyankha, "Ninakamba potuba tutu kuziko. Ninali kupunzisa muma sinagogi ndi mu tempele mwamene Ayuda amakumanilana pamodzi. Sininakambe mwakabisili. ²¹ Nichifukwa chani munifunsa? Funsani baja bamene benze bamvela vamene nenzokambapo. Onani aba banthu baziba vamene nenze nakamba." ²² Pamene Yesu anakamba izi zinthu, umozi wao pa alonda ana imilila pafupi anamumenyamo ndikunena kuti, "nanga ndiye mwamene ungayankile akulu ansembe?" ²³ Yesu anayankha, ngati nayankha kuipa, pelekani umboni pazoipa, koma ngati ni volungama, nichani chamene munimenyela?" ²⁴ koma Annasi anamutuma akali omangiwa kuli Kefasi mukulu wansembe. ²⁵ Koma Simon Petulo anayimilila ndi kuzifundisa eka. Ndi aba banthu bananena kuli iye, "kodi sindiwe mbali wa aja ophunzila ake?" anakana ndikunena, "sindine." ²⁶ Umozi waophunzila wa bakulu bansembe, wamene anali mubale wa uyu munthu wamene Petulo anajuba kutu, anakamba, "kodi sininakuone ndi iye mu munda na yeve?" ²⁷ Petulo anakana kachiwiri, ndipo pamene apo kombwe analila. ²⁸ Pamene apo anamutenga Yesu kuchokela kuli Kefasi ndikumu peleka kuli akulu la boma. Kunali kuseniseni, koma sanangene munyumba ya boma kuti asaziononge pamene akalibe kudya Pasaka. ²⁹ Koma Pilato anayenda kwaiwo ndi kubauza, "nanga chamene mumususila uyu munthu nichani?" ³⁰ Anamuyanka ndi kunena kulu iye, "ngati munthu uyu sinali oyipa, asemble sitinamutume kwa iye." ³¹ Pamwepo Pilato ananena kuli beve, "mutengeni imwe mweka, ndikumuweluzi kulinganiza na ulamulilo wanu." Ayuda ananena kuli iwo. "Sichili choenela kulinganila namalamulo kuti tipaye munthu alionse." ³² Anakamba ichi pakuti mau ya Yesu yafikilize chamene chinakambidwa kuti ni infa yabwanji yamene azafa. ³³ Koma Pilato anangena mumalo ya alonda a boma nafuti ndi kumuitana Yesu nakukamba kuli iye, "Kodi ndiwe mukulu waba Yuda?" ³⁴ Yesu ananena, "kodi ukamba kwaine weka, olo kapena banthu bena banakambapo kwa iye pali ine?" ³⁵ Pilato anayankha, "sindine muyud?, kodi ndine muyuda banthu bako ndi akulu ansembe anakupasa kwaine. Kodi unachita bwanji?" ³⁶ Yesu anayankha, "ufumu wanga si wamuno mu ziko. Ngati ufumu wanga unalimbari ya ziko lino, koma banchito banga ngati bamenya ngondo kuti musanipeleke kwa Ayuda. Koma manje ufumu wanga siuchoka pano." ³⁷ Pilato ananena kuli iye, "kodi ndiwe mfumu?" Yesu anayankha, "Wakamba kuti ndine mfumu. ninabadwila chamene ichi, koma nichifukwa chamene ichi nina bwela paziko kuti nikapeleke umboni wa choonadi. Aliwonse amene alikumbali ya choonadi amamvelela mau anga." ³⁸ Pilato ananena kuli iye, "Choonadi ni chichani?" pamene anakamba izi, anayenda kabiri kwa Ayuda naku auza, "sininapeze chifukwa chili chonse muli uyu munthu. ³⁹ Koma kulingana na mwambowatu nilinayo danga yomasulila umozi pa pasaka. Kodi mufuna nimasulile Mfumu

ya Ayuda kuli imwe?"⁴⁰ Ndiponso analila kachibili ni kunena, "siuyu munthu, koma Baraba." koma Baraba ni kawalala.

Chapter 19

¹ Pilato ana tenga Yesu naku kumukwapula. ² Basilikali bana panga chisote cha minga. Bana chiika pamutu wa Yesu naku muvalika chovala cha purple. ³ Bana bwela kuli eve naku kamba kuti, "Taonani, Mufumu wa ba Yuda!" Ndiponso bana mu menya. ⁴ Pamene apo Pilato ana enda panja nafuti naku bauza kuti, "Onani, nizamuleta panja kuli imwe kuti muzibe kuti uyu muntu sinina mupeze na mulandu." ⁵ Pamene paja Yesu anabwela panja, anavala chisote cha umfumu cha minga na chovala cha purple. Pilato anabauza kuti, "Onani, umuntu muntu ali apa!" ⁶ Pamene beve bakulu ba nsembe na ba silikali bana muona Yesu, bana punda naku kamba kuti, "Mupachikeni uyu muntu, mupachikeni uyu muntu." Pilato anabauza kuti, "Mutengeni imwe mweka mumupachike, chifukwa ine sinina mupeze na mulandu." ⁷ Ba Yuda bana muyanka kuti, "Ise tili nayo lamulo, kulingana na lamulo uyu ayenela kupaiwa chifukwa anali kukamba kuti ni Mwana wa Mulungu." ⁸ Pamene Pilato anamvela aya mau, ana gwiliwa na manta kwambili, ⁹ ana enda kungena mu malo yakulu ya boma nafuti naku mu-uza Yesu, "Nanga uchokela kuti?" Koma Yesu sana muyanke kalikonse. ¹⁰ Kukonkapo Pilato ana uza Yesu kuti, "Nanga nichani suniyanka? Nanga suziba kuti nili nazo mpavu zo kuchosa, na mpavu zo ku pachika?" ¹¹ Yesu anamuyanka kuti, "Ulibe mpavu zilizonse pali ine kapena chabe zija zamene zina pasiwa kuli iwe kuchokela kumwamba. Mwa ici, wamene anani peleka kuli iwe ndiye ali na chimo ikulu maningi." ¹² Pamene anamuyanka mau aya, Pilato anayesa ku mu chosa, koma ba Yuda bana punda, kukamba kuti, "ngati uza muchosa uyu muntu, ninshi sindiwe muzake wa Kaisala. Aliyense wamene amazipanga kunkala mfumu anyoza Kaisala." ¹³ Pamene Pilato anamvela mau aya, anamuleta Yesu panja naku munkalika pansu pa mupando wa chiweluzo mu malo oitaniwa kuti "Popita," koma mu chitundu cha chi Alamaiki bama itanamo kuti, "Gabata." ¹⁴ Manje inali ntawi ya kukonzekela kwa Pasaka, ntawi ya 12 koloko. Pilato anakamba ku-uza ba Yuda kuti, "Onani, uyu mfumu apa mfumu wanu!" ¹⁵ Bana punda naku kamba kuti, "Tiyeni naye uko, tiyeni naye uko; mupachikeni!" Pilato anabauza kuti, "Nanga nipachike mfumu yanu?" Bakulu ba nsembe bana yanka naku kamba kuti, "Ise tilibe mfumu koma chabe Kaisala." ¹⁶ Pamene apo Pilato anamupeleka Yesu kuli beve kuti bamu pachike. ¹⁷ Banamutenga Yesu, anachoka, ninshi anyamula mutanda wake, kuyenda kumalo oitaniwa kuti "Malo ya mafupa ya kumutu," yamene mu chitundu cha ku Aramaiki yaitaniwa kuti "Gologota." ¹⁸ Banamu pachika kwamene kuja, pamozi na bantu babili benangu, umozi ku kwanja ya kumanzele wina ku kwanja ya ku manja, Yesu pakati. ¹⁹ Pilato analembe chikwangwana naku chi ika pa mutanda. Pana lembewa mau yokamba kuti: YESU WA KU NAZALETI, MFUMU WA BA YUDA. ²⁰ Bambili ba Yuda bana belenga mau aya chifukwa chakuti malo yamene Yesu anapachikiwako yanali pafupi na Muzinda. Chikwangwana ichi china lembewa mu chilembewe cha chi Aramaki, Latini, na chi Giliki. ²¹ Pamene apo bakulu ba nsembe ba a Yuda bana uza Pilato kuti, "Osalembe kuti, 'Mfumu ya ba Yuda,' koma mulembe kuti, 'Uyu anali kukamba kuti, 'Ine ndine mfumu ya ba Yuda.'" ²² Pilato ana bayanka kuti, "Chamene ine nalemba nalemba." ²³ Pamene basilikali banamu pachika Yesu, bana tenga vovala vake, banavigabana muvigabo vi nai, aliyense pali beve anatengapo chimozi; na chovala chovala pamwamba. Koma chovala chamene ichi chakunja chinalibe joini, chotungiwa mbali imozi chabe kuchokela pamwamba. ²⁴ Bana uzana beka kuti, "Osati tichingambe chovala ichi, koma tiyeni titeye njuga kuti tizibe wamene azachitenga." Ichi chinachitika kuti mau yakwanilisike yolembewa yamene yakamba kuti, "Bana gabana vovala vanga pakati pabo naku chita kuteya njuga chifukwa cha vovala vanga." Ichi nichamene ba silikali bana chita. ²⁵ Manje bamene bana imilila pafupi na mutanda wa Yesu banali bamaike bake, ba kalongosi ba bamai bake, Maria mukai wa Klopas, na Maria Madalena. ²⁶ Pamene Yesu anaona bamai bake na opunzila wake wamene anali kukonda anaimilila pafupi, ana uza ba mai bake kuti, "Amai, onani, mwana wanu uyo!" ²⁷ Anauza uja opunzila wake kuti, "Ona, bamai bako!" Kuchokela pamene apo uja opunzila anaba tenga kuba peleka kunyumba kwake. ²⁸ Kuchokela apa, pamene anaziba kuti ntawi yakwana yamene vonse vina kwanilisiwa na kuti malemba yakwanilisiwe, Yesu anakamba kuti, "Namvela njota." ²⁹ Ka gubu kamene kanali na vinyo vosasa kanaikiwa paja, banatenga tonje yozula na vinyo vosasa pa ndodo ya hisopo na kuimya kupeleka kukamwa kwake. ³⁰ Pamene Yesu ana mwamo vinyo vosasa, anakamba kuti, "Chasilizika." Anagwedesa mutu wake na kupeleka muzimu. ³¹ Pamene apo ba Yuda, chifukwa iyi inali siku yokonzekela, mwa ichi ma tupi siyanga nkale pa mutanda pa ntawi ya Sabata (chifukwa ija Sabata inali yolemekezeka maningi), bana pempa Pilato kuti baba tyole mendo naku bachosapo. ³² Pamene apo ba silikali banabwela naku tyola mendo ya uja oyamba pamutanda na ya uja okonkapo wamene ana pachikiwa pamozi na Yesu. ³³ Pamene bana fika pali Yesu, bana ona kuti anamwalila kudala, mwa ichi sibana mutyole mendo. ³⁴ Koma, umozi pali basilikali anamu lasa lupenga kumbali, pamene apo kuna choka magari na manzi. ³⁵ Wamene anaona ivi apeleka umboni, na umboni wake niwa zo-ona. Aziba kuti wamene akamba nivazooni kuti mukulupilile naimwe. ³⁶ Chifukwa ivi vintu vinachitika kuti malemba yakwanisiwe, "Kulibe fupa yake ili yonse yamene izapwanyika." ³⁷ Nafuti, mau yena yakamba kuti, "Bazamu yangana wamene banalasa." ³⁸

Kuchoka ivi vintu, Yosefe waku Alimatiya, chifukwa chakuti anali opunzila wa Yesu (koma mu chisinsi chifukwa anali kuyopa ba Yuda), anapempa kuli Pilato kuti atenge tupi ya Yesu. Pilato anamuvomelesa. Kuchoka apa Yosefe anabwela nakutenga tupi. ³⁹ Nikodemas na eve anabwela, wamene anabwela kuli Yesu poyamba usiku. Analeta vosiyana-siyana monga myrrh na aloe, yokwanila monga ma lita yali hundredi. ⁴⁰ Pamene apa banatenga tupi ya Yesu na kui ika mu vovala va lineni na vonunkila, monga mwamene chinalili kunkalila ku mwambo wa ba Yuda pa kuika mutembo mu manda. ⁴¹ Manje mu malo mwamene anapachikiwa panali munda; ndipo mu munda uja munali manda ya sopano yamene sibana ikemo muntu aliyense. ⁴² Chifukwa inali siku ya kukonzekela kwa ba Yuda koma futi manda yanali pafupi, banaika tupi ya Yesu.

Chapter 20

¹ Kuseniseni mukuyamba kwa sabata, pamene kunali ko fipa, Mariya Magadalena anayenda kumanda ndipo anaona chimwala ni chochosewa pa manda. ² Anamanga nakuyenda kuli Simoni Petulo nakuli wina ophunzila wamene Yesu enzokonda, naku bauza ati, "Ba muchosako Ambuye mu manda ndipo sitiziba kwamene bamufaaka." ³ Petulo nabenangu bopunzila baake banachoka, bana yenda ku manda, ⁴ Bana tamanga pamozi, ndipo wina opunzila anamangisa kuchila Petulo nakufika ku manda musanga. ⁵ Ndipo pamene anabelama anaona nyula yankala, koma sanangene mo mukati. ⁶ Simoni Petulo pambuyo pake anafika nongena mumanda. Anaona nyula ili pansi yankala ⁷ Na nyula yenze pamutu wake. Sinankhale na manyula koma yenze yopetewa pamalo payeka. ⁸ Manje winangu ophunzila, uja ana fika musanga kumanda, nayeve ana'ngena, ndi kuona naku kukulupilila. ⁹ Kufikila ija ntawi sibanazibe malembo kuti azawuka kuwokufa. ¹⁰ Ndipo bopunzila bana bwelele ku nyumba nafuti. ¹¹ koma Maria enze ana yimlila panja alila. Pe'anzo'lila, ana'ngena mu'manada. ¹² ana'ona ba ngelo babili banavala voyela, wina anankala kumutu wina kumendo, panali tupi yo gona ya Yesu. ¹³ Bana kamba kwaeve, "Mukazi, mulila chani?" Ana bauza, "Chifukwa batenga Ambuye, ndipo siniziba kwamene bamufaka." ¹⁴ Pamene ana kamba izi, ana pindamuka naku ona Yesu ayimilila paja, koma sanazibe kuti ni Yesu anayimilila. ¹⁵ Yesu anakamba kwa iye, "Muzimai ulila chani? nindani wamene usakila muno?" Anaganiza kuti ni mulimi wa munda, ndipo anamuza, "Ambuye, ngati mwamutenga, niwuzeni kwamene mwa mufaka, ni zamuchosako." ¹⁶ Yesu ana muza, "Mariya." Ana pindamuka, ndipo ana muza muchi Aramaika, "Rabboni" (kutantauza "Mupunzisi") ¹⁷ Yesu ana muza iye, "Osanigwila, nikalibe kuyenda kumwamba kuli ba Tate, koma yenda ku'abale anga naku'bauza ati niku yenda ku mwanba kwa Tate wanga ndi Tate wanu, Na Mulungu wanga ndi Mulungu wanu." ¹⁸ Mariya Magadalene ana bwela na ku bauza bophunzila ati, "Namuona Ambuye," ndipo anakamba izii kwaeve. ¹⁹ Pamene mumazulo unafika, siku ija, siku yoyamba ya sabata, ndipo visiko kunali bophunzila vinali vo valiwa kuyopa Ayuda, Yesu ana bwela ayimilila pakati pao naku bawuza, "Mutendere kwa inu." ²⁰ Pamene ana kamba ivi, ana ba langiza manja yake na kumbali kwake. Bophunzila bana muona Yesu, ndipo bana kondwela ²¹ Yesu anabauza nafuti, "Mutendere kwainu. Mwamene Atate ananitungai, naine nikutumani." ²² Pamene Yesu anakamba izi anaba pemela mpepo na ku'kamba kuli beve, "Pokelelani Muzimu Oyela." ²³ Ngati mwakululukila machimo yamuntu aliense, azakhulukidwa; ndipo alionse wamene simunakululukila machimo yake, yazasungika. ²⁴ Thomasi, umozi wa bopunzila, wotaniwa Didimusi, sanalipo pamene Yesu anabwela. ²⁵ Bena bophunzila pa nthamwe inangu anamuza iye, "Tabaona Ambuye." Anakamba kwa iye, koma chabe nikaona mu'manja yake navibala vamisomali, na ku yika manja yanga pa vibala va misomali, nakufaka manja yanga kumbali yake, ndiye pamene nizakupilila." ²⁶ Panapita masiku eyiti (8) bophunzila bake banali mukati na futi, ndipo Tomasi anali nabo. Yesu ana bwela ninshi chiseko nicho valindwa, anayimilila pakati kao nakunena ati, "Mutendere unkale nainu." ²⁷ Ndipo analankula kuli Thomasi, "Fikiza pano vikumo vako, ndipo uzaona manja yanga, fikisa kwanja kwako uyike kumbali yanga, usankhale wosa khulupilirila koma wokhulupilila. ²⁸ Thomasi anayanka nokambaati kwaiye, "Ambuye wanga ndi Mulungu wanga." ²⁹ Yesu anakamba kwa iye ati, "Chifukwa waniona wakulupilila. Wodala ndi wonsa amene sananione koma akhulupilila." ³⁰ Manje Yesu anachita zizindikilo zambili pamaso pa bophunzila bake, zizindikilo zamene sizinalembedwa mubooku, ³¹ koma izi zalembedwa kuti mukulupilile ati Yesu ni Kristu, Mwana wa Mulungu, ndi kuti uka kulupilila, unkhale na moyo muzina yake.

Chapter 21

¹ Pamene vinasila ivi vintu Yesu anaonekela nafuti kuli bopunzila bake pa mumana wa Tibelias. Iyi ndiye njila yamene anaonekela: ² Simoni Petulo anali pamozi na Tomasi oitaniwa kuti Didimas, Nataniyeli ochokela ku Kana mu Galileya, bana ba Zebedi, na babili benangu bopunzila ba Yesu. ³ Simoni Petulo anakamba kuli beve kuti, "Niyenda kukasha nsomba." Banamu uza kuti, "Naise, kansi, tikukonka." Bana enda naku kwela mu bwato, koma sibana gwileko kali konse usiku onse. ⁴ Manje, pamene kunali kuseneni-kudala, Yesu anaimilila ku mbali kwa mumana, koma opunzila bake sibana zibe kuti ni Yesu. ⁵ Yesu anakamba nabo kuti, "Imwe bafana, nanga muli nacho cha kudya chili chonse?" Bana yanka nakumba kuti, "Iyayi." ⁶ Ana bauza kuti, "Ponyani nsumbo zanu ku zanja la manja kwa bwato, ndipo muzapezako nsomba." Bana ponya nsumbo yabo ndipo banakangiwa kui donsa chifukwa chakuti munali nsomba zambili maningi. ⁷ Ndipo uja opunzila wa Yesu wamene Yesu anali kumukonda anauza Petulo kuti, "Ni Ambuye." Pamene Simoni Petulo anamvela kuti banali niba Mbuye, anamangilila chovola chakunja (Chifukwa anali chintako), nakuziponya mu mumana. ⁸ Bopunzila baja benangu banabwela mu bwato (chifukwa sibanalali kutali na kunja kwa manzi, kulingana monga ma kilomita yali naini), banali kudonsa nsumbo yozula na nsomba. ⁹ Pamene banachoka kufika panja pa mumana, banaona mulilo wamalasha na nsomba zili pamulilo, na mukate. ¹⁰ Yesu anabauza kuti, "Letanikoni nsomba zinangu zamene mwagwila." ¹¹ Simoni Petulo ana enda naku kadonsa nsumbo kuileta kunja kwa manzi, yozula na nsomba zikulu-zikulu, zokwanila 153, ngankale kuti zinali zopaka mutundu uyu, nsumbo si-inangambike. ¹² Yesu anabauza kuyi, "bwelani mudye chakudya chakuseni." Koma kulibe opunzila aliyense wamene anazikosesa kuti amufunse kuti, "Nanga ndiwe ndani?" Bonse banaziba kuti eve ni Ambuye. ¹³ Yesu anabwela, nakutenga mukate, nakubapasa, na nsomba pamozi. ¹⁴ Ichi chinali ka chitatu kamene Yesu anaonekela ku bopunzila bake kuchokela pamene anauka ku bakufa. ¹⁵ Pamene banasiliza kudya chakudya, Yesu anauza Simoni Petulo kuti, "Simoni mwana wa Yohane, nanga unikonda kuchila aba bonse? Petulo anayanka kuti, "Nizo-ona Ambuye, naimwe muziba kuti nikukondani." Yesu anamu-uza kuti, "Pasa chakudya tubana twa mbelele twanga." ¹⁶ Anamu-uza nafuti kuti, "Simoni mwana wa Yohane, mwati unikonda ine?" Petulo anamuyanka kuti, "Zo-ona Ambuye, muziba kuti nikukondani." Yesu anakamba kuti, "Samalila mbelele zanga." ¹⁷ Anamu-uza nafuti kachitatu kuti, "Simoni mwana wa Yohane, mwati unikonda iwe?" Petulo anamvesa chifundo chifukwa Yesu anamufunsa katatu konse kuti, "Mwati unikonda iwe" Anamu-uza kuti, "Ambuye, muziba vintu vonse, muziba kuti nikukondani omwe." Yesu anamu-uza kuti, "Dyesa mbelele zanga." ¹⁸ Zo-ona, zo-ona, niku uza iwe, pamene unali mufana, unali kuzivalika weka naku yenda kuli konse kwamene wafuna, koma pamene ukota, uzatambasula manja yako, ndiponso muntu winangu azakuvalika iwe naku kupeleka kwamene iwe suzafuna kuti uyendeko. ¹⁹ Koma Yesu anakamba ivi kuti aonese njila yamene Petulo azamwalilamo ku ulemelelo wa Mulungu. Pamene anasiliza kukamba ivi, anamu uza Petulo kuti, "Nikonke ine." ²⁰ Petulo anapindamuka naku ona uja opunzila wa Yesu wamene Yesu anali kukonda abakonka, wamene anasamila Yesu pamene banali kudya chakudya cha usiku wamene anakamba kuti, "Ambuye, ni-uti wamene azakupelekani imwe?" ²¹ Petulo anamu ona naku uza Yesu kuti, "Ambuye, nanga uyu azachita chani kansi?" ²² Yesu anamu yanka kuti, "Nanga ngati nifuna kuti ankale mpaka ine nikabwele futi, chizankala bwanji kuli iwe? Tiye nikonke." ²³ Kukamba uku kunamveka kuli bopunzila bonse, kukamba kuti uja opunzila wa Yesu sazakamwalila. Koma Yesu sanamu-uze Petulo kuti opunzila uja saza kamwalila, koma, "nanga ngati nafuna kuti ankale namoyo mpaka ine nikabwele, chizankala bwanji kuli iwe nanga?" ²⁴ Uyu ndiye opunzila wamene apeleka umboni pali ivi vintu, wamene analemba ivi vintu, ndipo tiziba kuti umboni wake niwa zo-ona. ²⁵ Kuli vambili vamene Yesu anachita. Asembe ivi vintu vinalembewa, niganizila kuti ma buku yamene yangalembewe siyangakwane muziko ya pansi.

Acts

Chapter 1

¹ Book yakudala yamene ninalemba, Fiyofilisa, inakamba vonse vamene Yesu anayamba kuchita nakupunzisa, ² mpaka ija siku yamene analandiliwa ku mwamba. Ivi venzeli pambuyo pamene anapasa lamulo kupitila mwa Mzimu Woyela kuli ma apostoli bamene anasanka. ³ Pambuyo paku vutisiwa kwake, anazilangiza wamoyo kuli beve na umboni osashushika. Pamasiku yo kwanila 40 enzeli ku onekela kuli beve, ndipo anakamba za ufumu wa Mulungu. ⁴ Pamene enzeli kusunghana pamozi nabeve, anabalamulila kuti basachoke mu Yelusalemu, koma

kuti bayembekezele lonjezo ya Batate, yamene, banakamba, "Munavela kuchokela kuli ine ⁵ kuti Yohane zoona anali kubatiza na manzi, koma muzabatiziwa mu M'zimu Oyela mu masiku yang'ono." ⁶ Pamene banakumana pamozi banamufunsa, "Ambuye, kodi iyi ndiye nthawi yamene muzabwezela ufumu wa Israeli?" ⁷ Anakamba kuli beve, "Sindimwe mufunikila kuziba nthawi nangu nyengo yamene Batate banaika mwa mphamvu yabo." ⁸ Koma muzalandila mphamvu, pamene Muzimu Oyela azabwela pa imwe, ndipo muzankhala mboni zanga mu Yerusalemu namu Yudeya monse namu Samaria, nakosilizila kwa chalo." ⁹ Pamene Ambuye Yesu anakamba ivi vinthu, pamene beve benzeli kuyangana kumwamba, ananyamuliwa kuyenda kumwamba, na kumbi inamubisa kumenso yabo. ¹⁰ Pamene benzeli ku yanganisisa kumwamba pamene enzo yenda, Mosayembekezela, bamuna babili banaimilila pambali pabeve muli vovala voyela. ¹¹ Banakamba ati, "Imwe bamuna baku Galileya, ni chifukwa chani muli imilile apa muyangana kumwamba? Uyu Yesu wamene anayenda ku mwamba azakabwela na futi chimozi -mozi monga mwamene munamuonela kuyenda kumwamba." ¹² banabwelela ku Yerusalemu kuchokela pa lupili ya Olivu, yamene ili pafupi na Yerusalemu, mutunda ovomelezeka pa sabata. ¹³ Pamene banafika, banayenda mu chipinda chapamwamba, mwamene benzeli ku nkala. Panali Petulo, Yohane, Yakobo, Ndeleya, Philipo, Thomasi, Batlomeyo, Mateyo, Yakobo mwana wa Aliphasi, Simoni mu Ziloti, na Yudasi mwana wa Yakobo. ¹⁴ Banali bogwilizana pamozi bonse, pamene banapitiliza kupemphela maningi. Ku ikilapo panali futi bazimai, Maria mai wake wa Yesu, na babale bake. ¹⁵ Mumasiku yamene yaja Petulo anabwela nakuimilila pakati pa babale, bantu bokwanila ngati 120, nobwela ku kamba ati, ¹⁶ "Abale, chenzeli chofunikila kuti malemba yakwanilisike, yamene Muzimu oyela anakamba kudala kupitila mukamwa mwa Davide pa nkhanu ya Yudasi, wamene anasogolela baja bamene bana manga Yesu. ¹⁷ Anali umozi wathu ndipo analandila gawo yake ya uno utumiki." ¹⁸ (Manje uyu mwamuna anagula munda nandalama zamene analandila mu umambala wake, ndipo pamene apo anagwa kuyambila mutu, na thupi yake inaseguka chifukwa cho pholeka, namatumbo yake yonse yanataika panja. ¹⁹ Bonse bonkhala mu Yerusalemu banamvela pali ivi, ndipo banaitana munda uja mucitundu cao "Akeldama," ndiyekuti "Munda wa Magazi.") ²⁰ Cifukwa nicholembewa mu buku yama Salimo, 'Lekani munda wake unkhale owonongedwa, nakuti musavomeleze aliyense kuti ankhalemo'; 'Lekani munthu winagu atenge mupando wake wausongoleli.' ²¹ Nichofunikila, chifukwa chake, kuti umozi pali ba muna wamene anatikonkha nthawi zonse Ambuye Yesu anabwela nakuchoka pakati pathu, ²² kuyambila ku ubatizo wa Yohane kufikila siku yamene anayenda kumwamba kuchoka pali ise, afunika ankhale boni naise pa kuuka kwake." ²³ Banapeleka bamuna ba bili, Yosefe oitaniwa Barsabasi, wamene anali anali kuitaniwanso kuti Jusitasi, na Matiyasi ²⁴ Banapemphela nokamba ati, "Imwe, Ambuye, muziba mitima ya banthu bonse, ndipo woneselani kuti nindani pakati pali babili aba wamene mwasankha ²⁵ kuti atenge malo mu utumiki wa apositoli kuchokela kuli Yudasi wamene anachoka kuyenda munjila zake." ²⁶ Banachita masankho pali beve, ndipo kusankha kunagwela pali Matiyasi ndipo banamupendelapo pali ma apositozi bali 11.

Chapter 2

¹ Pamene siku ya Pentekosti inafika, banali pamozi bonse pa malo yamozi. ² Mosayembekezela kunabwela kuchoka kumwamba kumveka ngati chimphempo cha mphamvu, nozula mu nyumba mwamene banankala. ³ Panaonekela pali beve malilime monga ya mulilo yamene yanapasiwa, ndipo yanankhala pali aliyense. ⁴ Bonse banazulisiwa na Muzimu Oyela noyamba kukamba vitundu vinangu, mwamene Muzimu anabapasila kuti akambe. ⁵ Manje kwenzeli ba Yuda benzo nkhalu mu Yelusalemu, bamuna bali na umulungu, kucokela ku calo ciliconse cili pa ziko la pansi. ⁶ Pamene chongo ichi chinaveka, banthu bambili banabwela pa mozi ndipo banasokonezeka cifukwa cakuti aliyense anavela vama benzili kukamba mucitundu cawo. ⁷ Banadabwa ndipo banadabwa maningi; nokamba kuti, "Zoonu, nanga aba bonse bamene bali kukamba sibaku Galiliya?" ⁸ Cifukwa nicanu ise tibamvela, aliyense mucitundu cathu camene tinabadwilamo? ⁹ Patianzi, Medesi, na Elamitesi, nabaja bamene bankhala ku Mesopotamia, mu Yudeya na Kapadosia mu Pontasi na Azia, ¹⁰ mu Phrigiya na Pamphilia, mu Aigupto na mbali zina za Libiya ku Sailini na balendo bocokela ku Roma, ¹¹ Ayuda nabaja banatembenukila ku ciyuda, kretanzi, na Arabianzi, tibamvela kukamba muvitundu vathu pa zinchito za pamvu za Mulungu. ¹² Bonse banadabwa ndipo banadabwa maningi; banakambisana beka beka kuti, nanga ici citanthauza cani?" ¹³ But binangu banabaseka nokamba ati, "bakolewa na vinyu wa manje." ¹⁴ Koma Petulo anaimila pamozi nabali 11, nobwela upunda, nokamba kuti kuli beve, Ba muna baku Yudeya na bonse bamene munkhala mu Yelusalemu, lekani ici cizibike kuli imwe, mvesesani maningi ku mau yanga. ¹⁵ Cifukwa aba banthu sibanakolewe monga mwamene muganizila, ni 9 koloko yamumawa ino. ¹⁶ Koma ici ndiye camene cinakambiwa kupitila mu muneneri Jowelo: ¹⁷ 'Cizacitika mumasiku yosilizila; Mulungu akamba kuti, 'Nizatila Mzimu wanga pali banthu bonse. Bana banu ba muna naba kazi bazanenela, banyamata ba zaoona maso mphenya, ndipo madala bazalota maloto. ¹⁸ Naba nchito banga naba nchito ba kazi mumasiku ayo nizatila Muzimu wanga, ndipo bazanenela. ¹⁹ Nizaonesha zodabwisa mumulenga-lenga kumwamba ndipo zizindikilo pa ziko la pansi, magari, mulilo, nacusi cotikama. ²⁰ Zuba izasanduka kunkhala mudima ndipo na mwezi kukhala magari, pamene siku ikulu yokumbukilika ya Ambuye ikalibe kubwela. ²¹ Cizankhala kuti aliyense wamene ayitanina pa zina ya Ambuye azapulumsisiwa.' ²² Ba zibambo baku Israyeli, mvesesani aya mau: Yesu waku Nazareti, mwamuna oyikika na Mulungu kwa imwe na zocita zikulu-zikulu na zodabwisa na zizindikilo zamene Mulungu anacita kupitila mwa eve pakati panu, monga mwamene mwebene bake muzibila - ²³ cifukwa pulani yoikika na nzeli za Mulungu, anapelekewa kumwamba, ndipo imwe, kupitila mumanja ya bathu alibe lamulo, banamupacika nomupaya; ²⁴ wamene Mulungu ananyamula, pamene anamasula zobaba za imfa pa yeve, cifukwa sizenzi cokwanilisika kuti zimumangilile. ²⁵ Pakuti David akamba paliyeve, 'ninaona Ambuye nthawi zonse pamaso panga, cifukwa ali pa mbali ya kwanja kwanga kwaku raiti kuti ninacosewepo. ²⁶ Cifukwa caici mtima wanga unakondwela ndipo lulime yanga inakondwela. Nakuti thupi langa izankhala muciyembekezo. ²⁷ Cifukwa simuzasiya moyo wanga ku manda, kapena kuvomeleza Oyela wanu kuti awole. ²⁸ Munanibonesa njila za umoyo; muzanipanga kunkhala ozula na cimwemwe na pameso panu.' ²⁹ Ba bale banga, ninga kambe musimikiza pali tate wathu Davidi: anamwali ndipo anashikiwa, nakuti manda yake yali naife kufikila lelo. ³⁰ Cifukwa cake, anali mneneri ndipo anaziba kuti Mulungu analapa mwapangano kwa yeve, kuti azaika cimozi ca zipaso zake muthupi kunkhala pa m'mpando waufumu. ³¹ Anacibona ici ndipo anakamba za kuuka kwa Kristu, 'sanamutailila ku manda, kapena thupi yake kubola.' ³² Uyu Yesu-Mulungu anamuusha, wamene ise tonse ndise mboni. ³³ Cifukwa caici pakuukisiwa kunkhala kukwanja kwa ku raiti kwa Mulungu ndipo polandila Muzimu Woyela kucokela kwa aTate, wakhutula ici, camene mubona nakuvela. ³⁴ Davide sanayendeko ku mwamba, koma akamba ati, 'Ambuye anakamba kuti kuli Ambuye banga, "Nkhala pa kwanja paku raiti panga, ³⁵ panka nipange wadani bako codyakapo ca mendo yako." ³⁶ "Cifukwa ca ici, lekani nyumba yonse ya Israeli izibisise kuti Mulungu wapanga iye kunkhala Ambuye na Kristu, uyu Yesu wamene munapacika." ³⁷ Manje pamene banavela izi, wanalasiwa ku mtima kwabo, nokamba kwa Petulo na bonse ma apostoli, "ba Bale, tizacita bwanji?" ³⁸ Ndipo anakamba kwa beve, "Tembenukani na kubatiziwa, aliyense waimwe, muzina la Yesu Kristu kuti macimo yanu yakhululukiwe, ndipo muzalandila mpaso ya Mzimu Woyela. ³⁹ Kuli imwe kuli pangano ndipo ku bana banu na bonse bali kutali, na banthu bambili bamene Ambuye Mulungu azaitana." ⁴⁰ Namau inangu yambili anapelekela umboni nobalimbikisa; nokamba ati, "zipulumuseni kucoka kumubado oipa uyu." ⁴¹ Ndipo banalandila mau yake nobwela upatiziwa, ndipo ija siku myuyo ili 3000 inafakiwilako. ⁴² Banapitiliza mu ciphunziso na msonkhano wama apostoli, kunyemelana bredi na muma pemphelo. ⁴³ Mantha yanabwela yambwela pali moyo uliwonse, navodabwisa vambili na vizindikilo vinacitika nama apostoli. ⁴⁴ Bonse banakhulupilila banankhala ndipo benzeli nama kacitidwe kolingana, ⁴⁵ banagulisa katundu na cuma cao nobwela upasa aliyense kulinga navamene enzo funa aliyense. ⁴⁶ So Siku na siku banapitiliza nacolinga cimozi mu tempele, benzo nyemelana bredi mumanyumba, benzo gabana vakudya

mosangalala na m'mtima wozicepesa;⁴⁷ bana yamika Mulungu ndipo benze bokondewa na banthu bonse. Siku na siku Ambuye anafakilako kuli beve baja wamene wanapulumusiwa.

Chapter 3

¹ Manje Petulo na Yohane benzo yenda pa mwamba pa tempele pa nthawi ya pemphelo, pa nthawi ya 3 koloko mumazulu. ² Mudala winangu, olemala mendo kucokela pamene anabwadwa, benzo munyamula siku na siku nomugoneka pa ciseko capa tempele coitanidwa kuti Cokongola, kuti apempheko thandizo kuli baja benzo ngena mu tempele. ³ Pamene anaona Petulo na Yohane afuna kungena mu tempele, anapempha thandizo. ⁴ Petulo, kumuyanganisisa yeve, na Yohane, anakamba ati, "Yangana ise." ⁵ Olemela uja anabayangana beve, kuyembekezela kuti alandile cithu kuli beve. ⁶ Koma Petulo anakamba ati, Siliva na golide nilibe, koma camene nili naco, nikupasa. Muzina la Yesu Kristu waku Nazareti, yenda." ⁷ Petulo anamugwila pa kwanja, nomunyamula: ndipo pamene apo mendo yake na nkholola zake zinalandila mphamvu. ⁸ Kubwela ku jumpha, mudala olemala anaimilila noyamba kuyenda; anabwela angena na Petulo na Yohane mu tempele, kuyenda, nojumpha, noyamika Mulungu. ⁹ Banthu wonse anamuwona alikuyenda noyamika Mulungu. ¹⁰ Banabwela baziba ati niuja mudala wamene enzo nkhalala kulandila ndalama paciseko cokongola caku tempele, ndipo wanazhuzhiwa na kudabwa pacifukwa za mene zinacitika kwa iye. ¹¹ Pamene enzili gwililile kwa Petulo na Yohane, banthu bonse banathabila pamozi muma kholido yamene yaitawa modabwisa mwamukulu mwa Solomoni. ¹² Pamene Petulo anabona izi, anabayankha banthu, Imwe bamuna ba Israyeli, cifukwa nicani mudabwa? Cifukwa nicani mufaka menso pali ise, monga ngati namupanga kuti ayende namphamvu zathu kapene umulungu wathu? ¹³ Mulungu wa Abrahamu na Isaki, na Jakobo, Mulungu wa azitate bathu, alemekeza wanchito wake Yesu. Ndiye wamene munapeleka nomukana pamenso ya Pilato, pamene yeve anaganiza kuti amumasule. ¹⁴ Munakana Oyela na Wolungama, koma mumalo mwake munapempha kuti wopaya amasulidwe kwa imwe. ¹⁵ Munapaya Mfumu ya umoyo, wamene Mulungu anaukisa kucoka kwa akufa -ndipo ndise mboni pali ici. ¹⁶ Manje, mwacikhulupililo muzina lake -uyu munthu wamene muona noziba -zina yamene iyi inamupanga kunkhala olimba. Cikhulupililo camene cipitila mwa Yesu cinamupasa yeve umoyo uyu wokwanila mumeso mwanu imwe monse. ¹⁷ Manje, ba bale, niziwa kuti munacita kosaziba, monga mwamene wanacitila okulamililani. ¹⁸ Koma zinthu zamene Mulungu anazikambilatu kupitila mukwa mwa aneneli bonse, kuti Kristu afunika kuvutika, zakwanilisa manje. ¹⁹ Lapani, cifukwa cace, notembenuka, kuti mwacimo yanu yangacosewe, kuti nthawi zobvela zingabwele kucokela kupezekapo kwa Ambuye; ²⁰ nakuti angatume kristu wamene anasankhiwa kwa imwe, Yesu. ²¹ Ndiye wamene kumwamba kufunika kulandila paka nthawi yobwezewa vinthu vonse, pazamene Mulungu anakambapo kudala kupitila mukwama mwa aneneli bake oyela. ²² Mose zoona anakamba, 'Ambuye Mulungu azanyamula m'neneli monga ine kucokela pakati pa abale bako. Uzamvela zinthu zonse zamene yeve azakamba kwa iwe. ²³ Zizacitika kuti munthu aliyense wamene sazavelela kuli m'neneli azabonongewelatu pakati pa banthu.' ²⁴ Inde, bonse ba neneli kucokela kuli Samuyeli nabaja bamene anabwela pa mbuyo pake, banakambapo nopeleka cizibiso ca masiku aya. ²⁵ Ndimwe bana ba aneneli nabapangano yamene Mulungu anapangana namakolo yanu, monga anakambila kwa Abrahamu, 'mwa mbeu yako mabanja yonse pa calo yazadalisika.' ²⁶ Pamene Mulungu ananyamula wanchito wake, anamutuma kwa iwe poyamba, kuti akudalise iwe pakupindimula aliyense wa imwe kucoka kuzoipa zake."

Chapter 4

¹ Pamene Petulo na Yohane benzeli kukamba ku banthu, Asembe na kapitao wa mutepele naba saduki anabwela pa iwo. ² Banavutika kwambili cifukwa Petulo na Yohane benzo phunzisa banthu nolalikila mukuukisiwa kwa Yesu kucoka ku akufa. ³ Banabamanga nobafaka mu jele mphaka mumawa mwake, cifukwa kwenzeli kunayamba kufipa. ⁴ Koma banthu bambili bamene benze banavela uthenga anakhulupilila; ndipo namba ya bamuna banakhulupilila banali okwanila ngati faivi souzande. ⁵ Cinabwela cacitika pa siku yokonkhapo, kuti owalamulila, akulu amu pingo na wolamulila mu khoti banakumana pamozi mu Yelusalemu. ⁶ Annasi mukulu wa asembe enzelipo, na Kefasi, na Yohane na Alezanda nabonse benzeli abululu ba mkulu wa asembe. ⁷ Pamene anaika Petulo na Yohane pakati pawo, banafunsa, "Nimwa mphamvu zandani kapena muzina la ndani mwamene mwacita izi?" ⁸ Pamene apo Petulo, kuzuzhiwa na Mzimu Oyela, anakamba kwa beve, "Imwe olamulila wa banthu, na bakululu ba mpingo, ⁹ ngati ise lelo tifunsiwa pa kucita bwino kwa mudala odwala - nimunjila ya bwanji yamene anankhalilamo bwino?" ¹⁰ Lekani ici cizibike kuli imwe wonse na banthu wonse waku Israyeli, kuti mu zina la Yesu Kristu waku Nazareti, wamene munapacika, wamene Mulungu anausha kwa akufa -nimwa yeve kuti uyu mudala ayimilila pano pamaso panu wocilisiwa. ¹¹ Yesu Kristu nimwala wamene omanga munapepusa koma wamene wapangiwa mutu wamwala oyimililapo. ¹² Kulibe cipulumuso mu munthu winangu aliyense: cifukwa kulibe zina inangu pansi kumwamba, yamene inapasiwa pakati pa banthu, mwamene tifunika kupulumukila." ¹³ Manje pamene anaona kulimbika mtima kwa Petulo na Yohane, nozindikila kuti benzeli banthu cabe, banthu osaphunzila, wanadabwa, nobwela kuzindikila kuti Petulo na Yohane benzeli na Yesu. ¹⁴ Cifukwa anaona mudala wamene anacilisiwa oyimilila pamozi na beve, benzelibele ciliconse cokamba cosushana nabeve. ¹⁵ Koma pamene analamulila ma apostoji kuti acoke mu msokhano, banakambisana beke beke. ¹⁶ Anakamba kuti, tizacita bwanji na aba banthu? Ca zoona nicakuti codabwisa coonekelatu cacitika kupitila muli aba banthu bamene bankhala mu Yelusalemu; sitingacikane. ¹⁷ Koma kuti cisamveke maningi pakati pa banthu, tiyeni tibacenjeze kuti asakambenso na aliyense mu zina iyi." ¹⁸ Anaita Petulo na Yohane mukati nobalamulila kuti basakambenso kapena ku phunzisa mu zina la Yesu. ¹⁹ Koma Petulo na Yohane anayankha nokamba kwa beve, "Ngati nicabwino mumeso ya Mulungu kumvelela imwe kupambana Mulungu, weluzani. ²⁰ Sitingakwanise kuleka kukamba pavinthu vamene taona nakumvela." ²¹ Pobacenjezanso Petulo na Yohane, babatailila. Sibanapeze cifukwa camene angabapasile cilango, cifukwa banthu bonse benzo tamanda Mulungu pavamene vinacitika. ²² Mudala uja analandila milako yocilisiwa enze nazaka zopitilila 40. ²³ Pamene banabamasula, Petulo na Yohane anabwelela kuli banthu bawo nobauza vonse vamene akulu ansembe na akulu anabauza beve. ²⁴ Pamene banavela ici, banapunda pamozi kwa Mulungu nokamba, "Ambuye, imwe wamene anapanga kumwamba na pansi, na mumana, navonse vamene vilimo, ²⁵ imwe wamene mwa Mzimu Oyela, mwa mukamwa mwa atate bathu Davide kapolo wanu, anakamba, 'Nicifukwa nicani vialo va akunja akalipa, nakuti banthu aganiza vinthu vilibe nchito?' ²⁶ Mafumu yapaziko bazifaka pamozi, nabolamulila bakumana pamozi kusushana na Ambuye, na Kristu wake." ²⁷ Zoona, Herode na Pontiasi Pilato, pamozi na akunja na banthu ba Israeli, banakumana pamozi mutauni ino kusushana Yesu kapolo wanu oyela, wamene munazoya. ²⁸ Banakumana pamozi kucita zonse zamene kwanja kwanu nakufuna kwanu kunafuna kuti kucitike. ²⁹ Manje, Ambuye, onani cenjezo yabo ndipo mupase bakapolo banu kukamba mau anu namphamvu zonse. ³⁰ Kutu pamene mutambasula kwanja kwanu kuti mucilise, masaini na vodabwisa vingacitke kupitila muzina la Yesu kapolo wanu oyela." ³¹ Pamene banasiliza kupemphela, pamalo pamene banakumana pamozi panagwendezeka, ndipo bonse banazuzhiwa na Muzimu Oyela, ndipo banakamba mau ya Mulungu na mphamvu. ³² Namba ya banthu bambili bamene anakhulupilla benzeli na mtima na maganizo amoji: ndipo penzelibe nangu munthu umozi wamene anakamba kuti katundu wamene analibo wenzeli wake wake, mumalo mwake, banagabana wina na muzake. ³³ Namphamvu zambili ma apostoli benzo kamba za umboni wabo pa kuuka kwa Ambuye Yesu, ndipo cisomo cikulu cenzeli pali beve onse. ³⁴ Kwenzelibe nangu munthu umozi pakati pabo wamene anasoba kanthu, cifukwa baja bamene enzili na malo na manyumba banayagulisa ³⁵ noleta ndalama kucokela kuvamene banagulisa nozifaka pamendo yama apostoli. Ndipo kwezeli kupasa kuli okhulupilila aliyense, kulingana navamene enzofuna. ³⁶ Yosefe, mu Levi, munthu ocokela ku Saipulasi anapasiwa zina Banabasi nama apostoli (yamene itanthauza kuti mwana wa cilimbikiso). ³⁷ Yeve ponkhala namunda, anaagulisa noleta ndalama nozifaka pa mendo yama Apostoli.

Chapter 5

¹ Manje munthu winangu zina lake Ananiyasi, namukazi wake Saphira, anagulisa katundu wabo, ² nosungako ndalama zinangu (nakuti mukazi izoziba pali ici), noletako zinangu nozifaka pamendo yama apostoli. ³ Koma Petulo anakamba ati, "Ananiyasi, cifukwa nicani Satana wazula mumtima wako kuti uname boza kwa Mzimu woyela nakuti usungepo ndalama inangu yamalo yamene wagulisa?" ⁴ Pamene ukalibe kuyagulisa, kansi siyenzeli pansi paulamulilo wako? Cifukwa nicani waganiza pali ici mumtima mwako? Sunaname boza kubanthu, koma kuli Mulungu." ⁵ Pakumvela mau aya, Ananiyasi anagwa pansi nopeme kalasti. Ndipo mantha yakulu yanafika pali onse bamene banamvela izi. ⁶ Banyamata banabwela pasogolo nobwela umupomba, nobwelwela kumunyamula noyenda kumushika. ⁷ Pamene panapita 3 hours, mkazi wake anabwela, sanazibe camene cinabwela cacitika. ⁸ Petulo anakamba kwa yeve, "Niuza ngati munagulisa malo pa mtengo wa so." Anabwela akamba, "Eye, pamtengo wa so." ⁹ Pamene apo Petulo anabwela akamba kwa yeve ati, Cifukwa nicani mwangwilizana kuti muyese Mzimu wa Ambuye? Ona, mendo yabaja bamene ashika ba muna bako yali paciseko, ndipo bazakunyamula panja naiwe." ¹⁰ Pamene apo anabwela anagwela pamendo pake, nobwelo peme ka lasti, banyamata banangena nobwela kumupeza wakufa; banamunyamula noyenda kumushika pafupi namwamuna wake. ¹¹ Mantha yakulu yanabwela pa mupingo bonse, napali bonse bamene banamvela izi zinthu. ¹² Vizindikilo na vodabwisa vambili vezocitika pa banthu kupitila mumanja yama apostoli. Benzeli bonse pamozi mu kholido ya Solomoni. ¹³ Koma kwenzelibe aliyense enzeli olimbikila kuti abajoine, koma banabapasa ulemu banthu. ¹⁴ Nangu cenzeli so, bokhulupila benzo bwelelapo kwa Ambuye, bamuna na bakazi bambili, ¹⁵ paka benzo nyamula nabodwala mumiseu nobagoneka pama bedi napama cila, kuti pamene Petulo anabwela, cimvwili-mvwila cake cingagwele pali bena ba iwo. ¹⁶ Kunabwela futi banthu bambili kucoka kuma tauni yozungulila Yelusalemu, kubwelesa odwala nabonse bovutikila na vibanda voipa, ndipo bonse banacilisiwa. ¹⁷ Koma mukulu wa asembe ananyamuka, nabonse benzeli na yeve (yamene nigulu yama saduki); benzeli anakhala na jelasi ¹⁸ ndipo banagwila ma apostoli nobamanga nobafaka mundende za banthu bonse. ¹⁹ Koma panthawi ya usiku mu ngelo wa Ambuye anasegula viseko vamundende nobacosa panja, nobauza ati, ²⁰ "Yendani mukaimilile mu tempele nokamba kubanthu mau yonse ya umoyo uyu." ²¹ Pamene banamvela izi, banangena mu tempele camumawa ndipo anaphunzisa. Koma mukulu wa asembe anabwela, nabanja enzeli nayeve, noitanisa musonkhano pa mozi, bonse bakulu ba banthu baku Israyeli, nobatuma ku ndende kuti babwelese ma apostoli. ²² Koma ma ofisazi bamene anatumiwa sanabapezemo mu ndende, ndipo banabwelela nopeleka repoti, ²³ "Napeza ndende niyokhomewa bwino ndipo magadi oyimilila pa ciseko, koma pamene tinasegula, tinapeza mulibe munthu mukati." ²⁴ Manje pamene kaputeni wamu tempele na mukulu wa asembe banamvela mau aya, banadabwa maningi naveve pazamene zinacitika. ²⁵ Ndipo winangu anabwela abauza, "Bamuna bamene munafaka mundende ayimilila mu tempele ndipo aphunzisa anthu." ²⁶ Ndipo kaputeni anayenda nama ofisazi, nowabwelesa, kulibe viongo, cifukwa cakuti banayopa kuti anthu angabateme miala. ²⁷ Pamene banababwelesa, banaba nkhezika pali pa khanso. Mkulu wa asembe anabafunsa beve, ²⁸ kukamba kuti, "Tinakulamulilani maningi kuti musaphunzise muzina iyi, ndipo manje, mwazuzya Yelusalemu naziphunziso zanu, ndipo mufuna kuleta mwazi wa uyu munthu pa ise." ²⁹ Koma Petulo nama apostozi wanayankha, "Tifunika kumvelela Mulungu kupambana banthu.

³⁰ Mulungu waba tate bathu anamuusha Yesu, wamene munapaya pakumupacika pamtengo. ³¹ Mulungu anamukweza yeve kukwanja kwake kwa manja kunkhala mwana wa mfumu na mupulumusi, kupasa kutembenuka kuli Israyeli, naku khululukiwa kwa macimo. ³² Ndise mboni pali ivi vinthu, cimozi-mozi na Muzimu Oyela, wamene Mulungu anapasa kuli baja bamene amumvelela iye." ³³ Pamene ba khaso banamvela izi, banakalipa ndipo banafuna kupaya ma apostozi. ³⁴ Koma mfarisi zina yake Gamaliyeli, mphunzisi wama lamulo, wamene enze olemkezeka na banthu wonse, ananyamuka nola mulila kuti ma apostozi bapelekewe panja pakanthawi kang'ono. ³⁵ Ndipo anakamba kwa beve, "Ba muna ba Israyeli, mvesesani pazamene mukamba kucita kuli aba banthu. ³⁶ Panthawi yapita iyi, Teudasi ananyamuka nokamba kuti anali munthu wapandela, ndipo amuna ambiri, okwanila ngati 400 anamujoina iye. Anapaiwa, ndipo bonse benzomumvelela banamwazikana, nosililatu. ³⁷ Pamene anacoka uyu munthu, Yudasi waku Galileya ananyamuka pamasiku ya cibengelengo ndipo anadonsa banthu kukonkha yeve. Nayeve anaonongeka, nabonse benzo mumvelela banamwazikana. ³⁸ Manje nikamba kwa imwe, nkhalani kutali na aba banthu ndipo basiyeni, ngati iyi plani kapena nchito niya banthu, izagonjesewa. ³⁹ Koma ngati niya Mulungu, simuzakwanisa kubagonjesa; mungapeze kuti mwina mumenyana na Mulungu." Pamene apo anamvelela. ⁴⁰ Pamene apo anabaitana ma apostozi kuti bangene nobamenya nobalamulila kuti basakambe futi muzina la Yesu, nobwelo batailila. ⁴¹ Banacoka ku khanso wosangalala kuti banabelengelewa boyenela kuvesewa nsoni cifukwa ca Zina. ⁴² Pambuyo pake siku na siku, mu

tempele ndipo kucoka kunyumba noyenda nyumba kwinangu, banapitiliza kuphunzisa nolalikila Yesu kunkhala Kristu.

Chapter 6

¹ Manje mumasiku ayo, pamene namba ya ophunzila yenzo pakilako, dandaulo kucokela kuli Ayuda baku Gilisi anayamba kusushana na Aheberi, cifukwa akamukafilwa babo bacikazi benzo bapitilila mukagabidwa ka zakudya za siku na siku ² Bali 12 (Ma apostoji) anaitana gulupu ya ophunzila kuti abwele kuli beve ndipo anakamba, "Sikwabwino kuti ise tileke mau ya Mulungu kuti tiyambe kugaba vakudya. ³ Mufunika musankhe, abale, amuna bali 7 pakati panu, amuna bali na mbili yabwino, ozula na Mzimu na nzeru, bamene tizasankha pali iyi nchito. ⁴ Kwa ise, tizapitiliza muma pemphelo namu utumiki wa mau." ⁵ Kukamba kwao kuna kondwelesa gulupu yonse. So banasankha Stefano, mwamuna ozula nacikhulupililo na Mzimu Oyela, na Filipo, Prokoro, Nikanora, Timoni, Parmena na Nikolasi wosinthika wocokela ku Antioku. ⁶ Okhulupilila anabwelesa aba banthu kuli ma apostoji, wamene anapemphela noika manja yao pali beve. ⁷ So mau aMulungu yanayenda patali; ndipo namba ya ophunzila inapaka maningi mu Yelusalemu; ndipo namba ikulu ya asembe banankala osatila cikhulupililo. ⁸ Manje Stefano, ozula na cisomo na mphamvu, enzo cita zodabwisa zikulu na zioneselo pakati pa banthu. ⁹ Koma kunanyamuka banthu benangu benze baku sinagoge yoitaniwa sinagoge banthu omasulidwa, baku Sailini na Alekizanda, ndipo benagu wocokela ku Silisia na Azia. Aba banthu benzo cita musano na Stefano. ¹⁰ Koma sibanakwanise kusushana na nzeru na Mzimu wamene Stefano anakamba. ¹¹ So mwacisinsi banagomjesa banthu benangu kuti bakambe kuti, "Tamvela Stefano kukamba manyozo kuli Mose na Mulungu." ¹² Banatufya banthu, akulu, na alembi, ndipo aba banamufikila Stefano nomumanga nomuleta ku Khanso. ¹³ Banaleta mboni za boza, zamene zinakamba kuti, "Uyu munthu saleka kukamba mau yosusha aya malo oyela nalamulo. ¹⁴ Cifukwa ise tamumvela kukamba kuti uyu Yesu waku Nazareti azaononga aya malo nosintha myiambo ya Mose yamene yanapasiwa kwa ife." ¹⁵ Aliyense anakhala mu khanso anaika meso yeka pali yeve ndipo anaona kuti pa menso pake pali ngati pa menso pa mungelo.

Chapter 7

¹ Mukulu wa asembe anakamba kuti, Kansi izi zinthu nizazoon? ² Stefano anakamba kuti, "Abale naba tate onse, munivesese ine: Mulungu wa ulemelo anawonekel kuli batate bathu Abrahamu pamene enzeli ku Mesopotamia, pamene akalibe kukhala mu Harani; ³ anakamba kwa yeve, 'Siya malo yako na abululu bako, ndipo uyende kumalo yamene nizakuones.' ⁴ Ndipo anacoka pamalo ya Chaodiyanzi noyamba kunkhala mu Harani; kucoka apo, pamene atate bake anamwalila, Mulungu anamubwelesa mulalo aya, mwamene munkhala manje. ⁵ Sanapaseko malo yaliyonse kuli yeve, awe, ngankhale podyaka kwendo kwake. Koma analonjeza -ngankhale kuti Abrahamu analibe mwana -wamene angapase malo ngati katundu wake nabazukulu bake. ⁶ Mulungu enzo kamba nayeve socabe, kuti bazukulu bake azankhala pakanthawi muziko labene, nakuti bamene bankhalamo bazabapeleka mu ukapolo nobanzunza maningi zaka zili 400. ⁷ Ndipo nizaweluzi ziko yamene bazankhalamo mu ukapolo, Mulungu anakamba, ndipo vikasila ivi bazacokamo ndipo bazanipembeza ine mu malo yano. ⁸ Ndipo anapasa Abrahamu pangano ya mdulidwe, so Abrahamu anankhala tate wake wa Isaki nomucita mdulidwe pasiku ya namba 8; Isaki anakhala tate bake wa Yakobo, na Yakobo tate bake wabana bali 12. ⁹ Banali bali 12 banamucitila jelasi Yosefe nomugulisa ku Egypto, ndipo Mulungu enze nayeve, ¹⁰ nomucosa kumabvuto yake yonse, nomupasa cisomo na nzeru pamenso ya Farao, mfumu ya Egypto. Farao pamene apo anamupanga kunkhala gavana wa Egypto napanyumba pake ponse. ¹¹ Ndipo kunabwela njala pali ponse mu Egypto namu Kenani, namabvuto yakulu ndipobazitate bathu sibana peze vakudya. ¹² Koma pame Yakobo anamvela kuti kuli vakudya ku Egypto, anatuma makolo bathu nthawi yoyamba. ¹³ Nthawi yacibili Yosefe anazibonesela kuli ba bale bake; ndipo banja ya Yosefe inazibika kuli Farao. ¹⁴ Yosefe anatuma abale bake kuti abwelele kuti akauze Yakobo atate bake kuti babwele ku Egypto, pamozi nababululu bake bonse, banthu 75 pamozi. ¹⁵ So Yakobo anayenda ku Egypto, ndipo anamwalila, yeve namakolo yathu. ¹⁶ Banabapeleka ku Shekemu nobaika mu manda yamene Abrahamu anagula namutengo wa siliva kucokela ku bana ba muna ba Hama ku Shekemu. ¹⁷ Pamene nthawi yalonjezo inafika, lonjezo yamene Mulungu anapasa Abrahamu, banthu banakula nopaka mu Egypto, ¹⁸ paka mfumu inangu inayamba kulumulila mu Egypto, mfumu yamene sinazibe za Yosefe. ¹⁹ Mfumu yame iyi ina namiza banthu bathu nozunza makolo yanthu maningi, banapeleka bana babo kuciopyezo, kuyembekezela kuti bazapululumuka. ²⁰ Panthawi iyo nishi Mose wabadwa; enze okongolla pamenso ya Mulungu ndipo banamusamalila mwezi itatu munyumba ya atate bake. ²¹ Pamene banamutulusa panja, mwana mukazi wa Farao anamutenga nomukulisa ngati mwana wake. ²² Mose anaphunzira maphunziro yonse yaku Egypto; ndipo enze wamphamvu mu mau na zinchito zake. ²³ Koma pamene anakwanisa zaka 40, ananganiza mu mtima mwake kuti ayendele abale bake, bana ba Israyeli. ²⁴ Pakuona mu Israyeli anzunziwa, Mose anamuteteza iye nomubwezelako uja wamene anazunziwa pakumenya waku Egypto: ²⁵ ananganiza kuti abale bake azamvesesa kuti Mulungu kupyolela kukwanja kwake enzo bapulumusa, koma sibanamvesese. ²⁶ Pasiku yokonkhapo anabwela kuli ma Israyeli pamene benzo yambana; anayesesa kunkhazikisa mtendere pakati pao; nokamba ati, 'Azibambo, ndimwe paubululu; nicifukwa nicani muwonongana?' ²⁷ Koma uja analakwila muzake anamukankha, nokamba ati, wakupanga kunkhala olumulila nawoweluzi pali ise nindani? ²⁸ Ufuna unipaye mwamene unapayila waku Egypto mailo? ²⁹ Mose anathaba pamene anamvela izi; anankhala mulendo muziko ya Midiani, kwamene anankhala tate wa bana amuna abili. ³⁰ Pamene zaka 40 zinasila, mungelo anabonekela kwa yeve mucipululu ca Lupili ya Sinai, mucisamba coyaka mulilo. ³¹ Pamene Mose anabona mulilo, anadabwa pazamene anabona; ndipo pamene anafendela kuti abonesese, munacoka mau ya Ambuye, kunena, ³² Ndine Mulungu waba tate bako, Mulungu wa Abrahamu, na Isaki, na Yakobo.' Mose ananjenjeme ndipo sanafune futi kuyanganako. ³³ Ambuye anakamba kwa yeve ati, Bvula sapato zako, cifukwa malo yamene waimililapo nimalo yoyela. ³⁴ Nabonesesa maningi kuvutika kwa banthu banga mu Egypto; namvela kulila kwao, nabwela pansi kuzaba pulumusa; manje bwela nizakutuma ku Egypto. ³⁵ Uyu Mose wamene anakana, pamene anakamba ati, 'Nindani wamene anakupanga ulumulila na uweluzi?' -ndiye wamene Mulungu anatuma monga oweluzi na omasula. Mulungu anamutuma nakwanja kwa mngelo wamene anabonekela kuli Mose mumatepo. ³⁶ Mose anabasogolela kuwacosa mu Egypto, pambuyo po cita zodabwisa nazi zindikilo mu Egypto napa Mumana wa Matete, namucipululu munthawi ya zaka 40. ³⁷ Ni Mose wamene uyo wamene anakamba ku banthu ba Israyeli, 'Mulungu azanyamula mneneri pakati pa abale wanu, mneneri monga ine.' ³⁸ Uyu ndiye munthu wamene enzeli pa gulu mucipululu na mngero wamene anakamba naye Palupili ya Sinai. Uyu ndiye munthu wamene anali na azitate bathu; uyu ndiye munthu wamene analandila mau ya moyo kuti atipase ife. ³⁹ Uyu ndiye munthu wamene azitate bathu anakana kumumverela; anamukankhila patali kucoka kuli beve, ndipo kuti mumitima yabo banabwelele ku Egypto. ⁴⁰ Pali nthawi iyo banakamba kuli Aroni, 'Tipangile milungungu yamene izatisongolela. Cifukwa pali uyu Mose, wamene anatisogolela kucoka mu malo ya Egypto, sitiziba camene cacitika kuli yeve. ⁴¹ So banapanga ng'ombe

mumasiku ayo noleta sembe kuli mafano, nosangalala cifukwa ca nchito za manja yabo. ⁴² Koma Mulungu anaba pindimukila nobalekelela kuti bapembeze nthandala ku mwamba, monga cinalembwa mu buku ya aneneri, 'Kansi munapeleka kwa ine nyama zakufa na nsembe zaka zili 40 mucipululu, nyumba ya Israyeli?' ⁴³ Munalandila tenti ya Moleki na ntandala za mulungu Refani, na vithunzi-thunzi vamene munapanga kuti muvipembeze: ndipo nizakuperekani kutali kupitilila Babiloni.' ⁴⁴ Azitate bathubenze na tenti ya umboni mucipululu, monga mwamene Mulungu analamulila pamene anakamba na Mose, kuti ayipange monga patani yamene anaonapo. ⁴⁵ Iyi ndiye tenti yamene azitate bathu, pobwelela kwabo, yamene anabwelelsa kumalo pamozi na Yoshua. Ici cinacitika pamene analoba mukutenga malo yamene Mulungu anacosa pameso pa azitate bathu. Cinali socabe kufikila nthawi ya Davide, ⁴⁶ wamene anapeza cisomo mumeso ya Mulungu; anapempha kuti apeze malo okhalamo kwa Mulungu wa Yakobo. ⁴⁷ Koma Solomoni anamangila Mulungu Nyumba. ⁴⁸ Koma Olemekezeka sankhala munyumba zo pangidwa namanja; cili monga mwamene muneneri anenela, ⁴⁹ 'Kumwamba nipando wanga wacimfumu, pansi nipoponda mendo yanga. Kansi ni nyumba yabwanji yamene mungamangile ine? akamba Ambuye: olo yalikuti malo yopumulila yanga?' ⁵⁰ Kansi simanja yanga anapanga zonse izi?' ⁵¹ Imwe banthu amene muli oyuma na bosadulidwa mu mtima na mumatu, nthawi zonse mukana Muzimu Oyela; mucita mwamene azitate banu anacitila. ⁵² Nibati aneneri bamene azitate banu sibanzunze? Banapaya aneneri bamene anabwelelatu pamene Olungama sanabwele; ndipo manje mwankhala opacika na wopaya yeve futi, ⁵³ imwe banthu amene analndila lamulo yamene angelo anankhazikisa, koma simunaisunge." ⁵⁴ Manje pamene ma membala ba khanso banamvela izi, banakhuziwa ku mtima, ndipo banamulumila meno Stefano. ⁵⁵ Koma yeve kunkhala ozula na Mzimu Oyela, anayanganisisa kumwamba nowona ulemelo wa Mulungu; ndipo anaona Yesu oyimilila kukwanja kwa rayiti kwa Mulungu. ⁵⁶ Stefano anakamba ati, "Onani, niwona kumwamba koseguka, ndipo Mwana Mwamuna wa Munthu oyimilila kukwanja kwa rayiti kwa Mulungu," ⁵⁷ Koma ma membara ya khanso yanapunda maningi, noleka kumvera, nothamangila pali yeve pamozi; ⁵⁸ banamuponya panja pa tauni nomutema miala: ndipo wotambako banafaka vovala vabo vakunja pali munyamata oyitaniwa Sauli. ⁵⁹ Pamene benzo mutema miala Stefano, anapitiliza kuitana Ambuye kukamba kuti, "Ambuye Yesu, landilani mzimu wanga." ⁶⁰ Anagwada pansi nobwela kuitana maningi, "Ambuye, musasunge cimo iyi kuli beve." Pamene anakamba ivi, anamwalila.

Chapter 8

¹ Sauli anavomelezana nayo ifa yake. So mpingo unali ku Yelusame unayamba kusausidwa kwakukulu siku yamene iyo; ndipo okhulupirila anamwazikana ponse ponse kumizinda ya Yudeya na Samaria, kucoselako ma apostoji. ² Amuna ozipileka anamushika Stefano ndipo anamulila maningi yeve. ³ Koma Saulo ananzunza mpingo maningi; anayenda nyumba na nyumba nodosa amuna na akazi, nobafaka mu jele. ⁴ Koma okhulupilila amene anamwazikana anapitana-pita kulalikila mau. ⁵ Filipo anayenda ku tauni ya Samaria nobalalikila beve Kristu. ⁶ Pamene banthu bambiri banamvera nowona vizindikilo vamene Filipo anacita, banafakako nzelu pamozi kuzamene enzokamba. ⁷ Cikufakwa kucoka kubanhu ambili amene anali navo, mizimu yonyansa inacoka mopunda maningi; ndipo bambili ozizila naboalemala mendo anacilisiwa. ⁸ Ndipo mwenzeli cisangalalo cikulu mu tauni. ⁹ Koma mwenzeli munthu winangu mu tauni zina lake ni Simoni, wamene kumbuyo inzo citata vaufwiti; enzo badabwisa banthu baku Samaria, pamene enzo kamba kuti nimunthu ofunikila maningi. ¹⁰ Ba Samaria bonse, kucokela kumwana kufikila mukulu, enzno mufakila nzeru yeve; anakamba, "Uyu munthu ndiye ija mphambu ya Mulungu yamene iyitaniwa kuti Yaikulu." ¹¹ Anamumvelera yeve, cifukwa cakuti anabadabwisayeve kwa nthawi kwa nthawi itali na ufwiti ake. ¹² Koma pamene banakhulupila Filipo pazamene analalikila pa uthenga okamba paza ufumu wa Mulungu na zina ya Yesu Krsitu, anabatizika, amuna nabazimai nabo. ¹³ Ndipo Simoni nayeve anakhulupilila, anapitiliza kunkala na Filipo; pamene anabona visanzo na zocita zikulu kucitika, anadabwa. ¹⁴ Manje pamene ma apostoji banamvera kuti Samaria inlandila mau amulungu, anabatumizila Peturo na Yohane. ¹⁵ Pamene banabwela, anabapemphelela, kuti alandile Mzimu Oyela. ¹⁶ Cifukwa kufikila ija nthawi, Mzimu Oyela enze akalibe kubwela pali aliyense wa beve; benze banapatizika cabe mu zina la Ambuye Yesu. ¹⁷ Pamene apo Peturo na Yohane anafaka manja yabo pali beve, ndipo analandila Mzimu Oyela. ¹⁸ Manje pamene simoni anabona kuti Mzimu Oyea wapaswa kupitila mukuikapo manja yama apostozoi, anabwela abapasa ndalama. ¹⁹ Anabwela akamba ati "Ninepaseni izi mphamvu, naine, kuti aliyense wamene nizafakaka manja yanga payeve azalandil a Mzimu Oyela." ²⁰ Koma Peturo anakamba kwa yeve, leka siliva yako ibonongeke pamozi naiwe, cifukwa waganiza kuti ungalandile mphaso ya Mulungu nandalama. ²¹ Ulibe mbali pali ici, cifukwa mtimwa wako sulibwino na Mulungu. ²² Cifukwa caici tembenuka kuzoipa zako, ndipo upemphere kwa Ambuye, kuti mwina akukhululukile manganizo umumtima mwako. ²³ Cifukwa nabona kuti uli mu poisoni yalukhubwa ndi maunyolo ya ucimo." ²⁴ Simoni anayankha nokamba ati, Nipempherele kwa Ambuye, kuti visacitike kwa ine pavamene wakamba." ²⁵ Pamene Petro na Yohane anankhala na umboni nokamba mau ya Ambuye, anabwelela ku Yelusalemu; penzo yenda munjira, analalikila uthenga ku minzi yambili ya Asamaria. ²⁶ Manje mungelo wa Ambuye anakamba na Filipo kuti, "Nyamuka ndipo uyende kumazulo ku njila yamene icokela ku Yelusalemu kuyenda ku Gza." (Iyi njila ili mucipululu.) ²⁷ Ananyamuka noyenda. Onani apo, kunali munthu ocokela ku Ethiopia, olemkezeka wamene anali naulamulilo ukulu kuli mafumu, mkazi wa mfumu yama Ethiopians. Ndiye enzeli osunga ndalama za mkazi wa mfumu. Enzeli anabwela ku Yelusalemu kumbela ku pembeza. ²⁸ Enzo bwelelamo nishi wankhala mucikocikali, ndipo enzo belenga mneneri Yesaya. ²⁹ Mzimu unakamba kuti kwa Filipo, "Yenda pafupi nokhala pafupi na cikocikali." ³⁰ So Filipo anathamangila kuli yeve, nomumvera abalenga Yesaya mneneri, ndipo anakamba ati, "Kansi umvela vamene ubelenga?" ³¹ Mu Ethiopian anakamba ati, Ningamvele bwanji, koma kapena winangu anisogolele?" Anapempha Filipo kuti angene mucikocikali nonkhala nayeve. ³² Manje ndime ya mau yenzo belenga mu Ethiopian yenze iyi, "Anapelekewa ngati mberere kuyenda upaiwa; monga mwana wa mberere akhalila zii kuli uja wamene agela usako wake, sasegula pakamwa: ³³ Mukumupepusa ciweluzilo cake wacicosa: azakamba zamubado wake nindani? cifukwa umoyo wake unacosewa pa ziko lapansi." ³⁴ So uyu olemkezeka anafunsa Filipo, nokamba ati, nikupempha, nindani wamene mneneri akamba? Akamba zayeve olo munthu winangu?" ³⁵ Filipo anayamba kukamba; anayamba na mau yali mu Yesaya kulalikila pali Yesu kuli Yeve. ³⁶ Pamene anapitiliza kuyenda mnjila, anafika panali manzi; wolemekezeka anakamba ati, Ona pali manzi apa; cizanilesa kubatizika nicani?" ³⁷ (Filipo anakamba ati, ngati ukhulupilila na mtima wako bonse, ungabatiziwe." Olemkezeka anakamba ati, "Nikhulupilila kuti Yesu Kristu nimwana mwamuna wa Mulungu.") ³⁸ So mu Ethiopian analamulila kuti cikocikali kuti ci imilile. Banayenda mu manzi, bonse babili Filipo na wolemekezeka, ndipo Filipo anamubatiza yeve. ³⁹ Pamene banacoka mu manzi, Mzimu wa Ambuye unamutenga Filipo; wolemekezeka sanauone futi, ndipo anapitiliza na ulendo wake wosangalala. ⁴⁰ Koma Filipo anabonekela ku Azotasi. Anapitila ku mzinda wamene uja nolalikila uthenga kuma tauni yonse, mpaka anafika ku Sizalia.

Chapter 9

¹ Koma Sauli, akali kuyofya zopaya ophunzira ba Ambuye, anayenda kwa akulu asembe ² nomupempha makala yakuma sinagoge mu Damasiko, kuti ngati wapeza wina aliyense olondola Njira ya Chikristu, amena kapena azimai, ababwelese omangiwa ku Yelusalemu. ³ Pamene enzo yenda, cinacitika kuti pamene anafika pa fupi na Damasiko, mwazizi kunabonekela pali yeve laiti kucoka ku mwamba; ⁴ ndipo anagwa pansi novela mau kukamba kuti, "Sauli, Sauli, cifukwa nicanu unisauza ine?" ⁵ Sauli anayankha ati, "Ndimwe ndani, Ambuye? Ambuye anamuyankha ati, Ndine Yesu wamene usausa; ⁶ koma nyamuka ngena mu tauni, uzauziwa vamene ufunika kucita." ⁷ Bamuna banali nayeve anlibe cokamba, kumvela mau, koma osaona aliyense. ⁸ Sauli ananyamuka pansi, ndipo pamene anasegula menso, kulibe cili conse camene anaona; so banamugwila pa kwanja nomuleta mu Damasiko. ⁹ Pamasiku yatatu senzoona, ndipo sadye kapena kumwa kali konse. ¹⁰ Manje kunali ophunzira mu Damasiko zina lake Ananiya; ndipo Ambuye anakamba nayeve mu maso mphenya, "Ananiya." Ndipo anakamba ati, "Onani, Nilipano Ambuye." ¹¹ Ambuye anakamba nayeve, "Nyamuka, ndipo yenda munjila yamene iyitaniwa kuti Siteleti, ndipo pa nyumba ya Yudasi akafunse kuti ufuna mwamuna wamene acoka ku Tasasi oyitanidwa Sauli; cifukwa ali kupemphera; ¹² ndipo awona maso mphenya ya munthu zina lake ni Ananiya kubwela noyika manja pa iye, kuti ayangane futi." ¹³ Koma ananiya anayankha, "Ambuye, nemvera kuli ambili pali uyu munthu, kuwononga kwamene awononga ku banthu oyela ali ku Yelusalemu." ¹⁴ Ali na mphamvu kucoka kuli mkulu wa nsembe kuti amange aliyense wamene ayitana pa zina lanu." ¹⁵ Koma Ambuye anakamba ati kuli yeve, "Enda, cifukwa nicosebenzela canga co sankhika, kunyamula zina langa kuli akunja na mafumu na bana ba Israyeli; ¹⁶ cifukwa nizamubonesa mwamene afunika ku vutisiwa cifukwa ca zina langa." ¹⁷ So Ananiya anayenda, noloba munyumba. Pakuika manja yake pali yeve, anakamba ati, "Mubale Paul, Ambuye Yesu, wamene anabonekela kuli iwe pa njila pamene wenzobwela, anituma kuti uyangana futi ndipo ulandila Mzimu Oyela." ¹⁸ Pamene apo vinthu monga mamba vinacoka kucoka mu menso ya Sauli, ndipo anayangana; ananyamuka ndipo anabatizika; ¹⁹ ndipo anadya nonkhala na mphamvu. Anankala na omphunzira ku Damasiko pama siku ambili. ²⁰ Pa nthawi yamene iyo analalikila za Yesu mumasinagoge, kukamba kuti iye nimwana mwamuna wa Mulungu. ²¹ Bonse bamene anamumvela banadabwa nokamba kuti, "Kansi siuja wamene anabononga baja wamene anaitana pali iyi Zina? Ndipo abwela kuno kuti ababwelese womangidwa kuli mukulu wa nsembe." ²² Koma Sauli anankhala maningi namphamvu, ndipo analeta vuto pali ba Yuda amene enzo nkhalu mu Damasiko pakuwasimikizila kuti Jesu ni Kristu. ²³ Pamene panapita masiku ambili, Ayuda anapanga zakuti ba mupaye yeve. ²⁴ Koma plani yabo inazibika kuli Sauli. Banayanganila pa geti usiku na muzuba nausiku kuti bamupaye. ²⁵ Koma ophunzira bake banamutenga usiku nomupitisa kucipupa, kumupeleka pansi mu basiketi. ²⁶ Pamene anabwela ku Yelusalemu, Sauli anayesa kujoina ophunzira, koma bonse banamuyopa yeve, sabanakhulupilile kuti enzeli ophunzila. ²⁷ Koma Banabasi anamutenga nomupeleka kuli ma apostoji. Ndipo anabauza mwamene Sauli anabonele Ambuye pa njila nakuti Ambuye anakamba nayeve, namwamene Sauli analalikilila mwamphamvu muzina la Yesu ku Damasiko. ²⁸ Anayenda nayeve pamene benzongena nocoka mu Yelusalemu. Anakamba mwamphamvu muzina la Ambuye Yesu ²⁹ nokambilana na aYuda aCigiliki; koma banapitiliza kufuna kumupaya. ³⁰ Pamene abale banaziba pali ici, banamupeleka ku Sizelia nomutuma ku Tasisi. ³¹ So manje, mupingo monse mu Judeya, mu Galileya, mu unali namutendele ndipo unalimba; noyenda mukuyopa Ambuye ndiponso mucitonthozo ca Mzimu Oyela, mupingo unakula mu namba. ³² Manje cinabwela cacitika kuti, pamene Petro anapitamo muzinda bonse, anabwela kuli ba okhulupilila benzo nkhalu mu tauni ya Lida. ³³ Kuja anabwela apeza mwamuna winangu zina lake ni Aneyasi, wamene anali cigonele pabedi yake zaka 8, cifukwa enzeli olemala mendo. ³⁴ Petro anakamba kwa yeve kuti, "Aneyasi, Yesu Kristu akucilisa iwe. Nyamuka noyanzula bedi yako." Ndipo pamene apo ananyamuka. ³⁵ So aliyense wamene enzonkhala mu Lida namu Sharoni anamuona uja mwamuna ndipo anatembenukila kwa Ambuye. ³⁶ Manje kwenzeli ophunzira winangu ku Yopa zinalake ni Tabita, yamene itanthauza "Dokasi." Uyu mzimayi enzeli maningi wazinchito zabwino na zacifundo zamene anacitila osauka. ³⁷ Cinabwela cacitika kuti mumasiku ayo anadwala nomwalila; pamene banamusambika, banamugoneka mucipinda capamwamba. ³⁸ Cifukwa cakuti Lida yenzeli pafupi na Jopa, nakuti ophunzila banamvera kuti Petro enzeli kwamene kuja, banatumako bamuna babili kuli yeve, kumupempha, bwela kuno mosawaya-wayaya." ³⁹ Petro ananyamuka noyenda nabeve. Pamene anafika, banamupeleka mucipinda capamwamba. Ndipo wonse bazimayi ofedwa anayimilila pafupi nayeve nishi balila. ⁴⁰ Petro anabacosa panja bonse, anagwada pansi, nopemphela; nobwela upindimukila kuli thupi, anakamba ati, "Tabita, nyamuka." Anasegula menso yake, ndipo pamene anaona Petro ananyamuka nonkhala. ⁴¹ Petro anamugwila kwanja nomunyamula; ndipo pamene anaitana okhulupilila na azimai ofedwa, nomupeleka

kulibeve wamoyo.⁴² Iyi nkhani inazibika mu Yopa monse, ndipo banthu bambili anakhulupila mwa Ambuye.⁴³ Cinabwela cacitika kuti Petro anakhala masiku ambiri mu Yopa na mwamuna ocedwa Simoni, bopanga vikumba.

Chapter 10

¹ Manje kwanzeli mwamuna winangu mu tauni ya Sizelia, Koniliyasi zina lake, msilikali wamene enzo itanidwa msilikali waci Italiani. ² Enze mwamuna ozipeleka, wamene anapempheza Mulungu na banja yake yonse; anapeleka ndalama zambili kuli banthu baci Yuda ndipo nthawi zonse kupempela kwa Mulungu. ³ Panthawi ya 3 koloko mumazulo, anaona bwino-bwino mumaso mphenya mngelo wa Mulungu kubwela kwa iye. Mngelo anakamba kwa eve, ⁴ "Koniliyasi!" Koniliyasi anayangana mngelo ndipo anayopa maningi nokamba ati, "Nican, akulu?" Mngelo anakamba ati kwa yeve, "Mapemphelo yako napaso kuli osauka zayenda kumwamba munga sembe yokumbukilika kwa mu ulemelelo wa Mulungu. ⁵ Manje tuma wamuna ku tauni ya Yopa kuti wakabwelese mwamuna wocedwa Simoni oyitanidwa kuti Petro. ⁶ Ankhalala na opanga vikumba ocedwa Simoni, wamene nyumba yake ili mumbali yamumana." ⁷ Pamene mngelo anakamba nayeve anayenda, Koniliyasi anaitana banchito bake bamunyumba babili, namusilikali wamene enzo pembeza Mulungu pakati pa asilikali bamene benzo musebenzela yeve. ⁸ Koniliyasi anababuza wamene vinacitika ndipo anabatuma ku Yopa. ⁹ Manje pasiku yokonkhapo panthawi ya 12 koloko, pamene benzeli pa ulendo wao nishi bankhala pang'ono kufika mu tauni, Petro anayenda pamwamba panyumba kuyenda kupemphera. ¹⁰ Abwela amvera njala ndipo ezno funana wamene angadye, anpasiwa maso mphenya, ¹¹ ndipo anaona kumwamba kwaseguka nakontena inangu cucoka kumwamba, cinthu cinangu munga cinyula cikulu kubwela pansi, colekelelewa namakona yake yali 4. ¹² Muliceve mwenzili nyama zonse zosiyana siyana zamendo 4 navinthu voyenda pansi, nanyoni za mumwamba. ¹³ Pamene apo mau yanakamba nayeve: Nyamuka Petro, Paya nakudya." ¹⁴ Koma Petro anakamba ati, Osati so, Ambuye; cifukwa sininadyepo vinthu vilivonse vodesedwa." ¹⁵ Koma mau yanabwela kwa yeve futi kacibili: Camene Mulungu watubisa, osaciitana codesewa." ¹⁶ Ici cinacitika katatu; ndipo cikontena cinabwela cacosewapo pamene apo kubwelera kumwamba. ¹⁷ Manje pamene Petro enze akali osokonezeka camene masophenya yamene anaona camene yatanthauza, pamene apo, amuna bane Koniliyasi enze anatuma banimilila pa gate, nishi beze banafunsa njila yakunyumba. ¹⁸ Ndipo anaitana nofunsa ngati Simon, wamene enzoitaniwa Petro, ngati enzo nkhalala paja. ¹⁹ Petro nishi akali kunganiza za maso mphenya, Mzimu anakamba nayeve, ona, bamuna batatu basakila iwe. (Mau inangu yakamba ati, "bamuna babili akusali." olo "bamuna benangu bakusakila"). ²⁰ Nyamuka ndipo uyende nabeve. Osawaya waya kuyenda nabeve, cifukwa nabatuma." ²¹ So Petro anayenda kuli baja bamuna nokamba ati, Ndine wamene musakali. Mwabwelera cani?" ²² Banakamba ati, Musilikali ocedwa Koniliyasi, munthu wangwilo ndipo wamene apembeza Mulungu, ndipo muntundu bonse waba Yuda ukamba zabwino za yeve, anauzidwa namungelo woyela wa Mulungu kuti ayitane iwe ubwele kunyumba kwake, kuti amvere uthenga kucokela kwa iwe." ²³ So Petro anabaitana kuti bangena nonkhala nayeve. Pasiku yokonkhapo, ananyamuka noyenda nabeve, ndipo babale benangu cucoka ku Yopa anayenda nayeve. ²⁴ Pasiku yokokhapo anafika ku Sizeliya. Koniliyasi enzo bayembekezela beve; enza anaitana banja lake pamozi nabazake maningi. ²⁵ Cinabwela cacitika kuti pamene Petro anangena, Koniliyasi anakuma nayeve ndipo anamugwadila pamendo pake kuti amupembeze. ²⁶ Koma Petro anamuthandiza kunyamuka, nukamba ati, "Nyamuka! Naine ndine munthu." ²⁷ Pamene Petro enzo kamba nayeve, anangena nopeza banthu bambili basonkhana pamozi. ²⁸ Anakamba nabeve, "Imwe mweka muziba kuti silamulo kuti munthu waci Yuda angayanjane nabo olo kuyendela munthu ocokela kuziko kwinangu. Koma Mulungu wanionesa kuti sinifunika kuitana munthu aliyense wodesedwa. ²⁹ Cifukwa sinasushe pobwela, pamene ninatumiwa. So nikufunsa nican camene waniitana ine." ³⁰ Koniliyasi anakambaati, Masiku 4 yapita panthawi yamene ino, nenzo pemphera panthawi ya 3 koloko mumazulo munyumba mwanga; ndipo ona, munthu anaimilila pa maso panga mumalaya yowala. ³¹ Anakamba ati, 'Koniliyasi, pemphero yako yaveka kwa Mulungu, ndipo nsembe yako kuli osauka yakumbusa Mulungu pali iwe. ³² So tuma winangu ku Yopa, ndipo uyitana munthu ocedwa Simoni wamaene ayitaniwa kuti Petro. Ankhalala munyumba ya wopanga vikumba ocedwa Simoni, mumbali yamumana.' ³³ (Pamene apo ninakuitana. Ndiwe wabwino mtima kuti wabwela. Manje, tilipano tonse pamozi pamenso pa Mulungu, kuti timvele zonse zamene wauziwa na Ambuye kuti ukamba). ³⁴ Pamene apo Petro anabvula kamwa kake nokamba ati, "Zoonadi, naona kuti Mulungu satenga mbali yamuthu aliyense. ³⁵ Mmallo mwake, muziko iliyi yonse aliyense wamene amupembeza nocita nchito zacilungamo nowolandiliwa kwa yeve. ³⁶ Uziba uthenga wamene unatumiwa kuli banthu baki Israyeli, pamene ana naunsa za uthenga wabwino pazamutendele kupyiolela mwa Yesu Kristu, wamene ali Mbuye wa bonse - ³⁷ imwe mweka muziba pazamene zinacitika, zamene zinacitika mu Yudeya monse, kuyambila mu Galileya, utasila ubatizo wamene Yohane ana naunsa; ³⁸ zocitika zokhuza Yesu waku Nazareti, mwamene Mulungu anamuzozela na Mzimu Oyela na mphamvu. Anayenda kucita zabwino nocilisa bonse benzeli opondelezedwa na satana, cifukwa Mulungu enzeli nayeve. ³⁹ Ndise mboni pazonse zamene anacita muziko la Ayuda namu Yelusalemu -uyu Yesu wamene anapaya, pakumupacika pa mutengo. ⁴⁰ Uyu munthu

Mulungu anamubusha pasiku yanamba 3 nomupasa kuti azibike,⁴¹ osati kubanthu bonse, koma kuli mboni zamene zinasankhika kale na Mulungu -ise bamene, wamene tinadya nakumwa naye pamene anauka kwa akufa.⁴² Anatilamulila kuti tilalikile ku banthu nopelekela umboni kuti uyu ndiye wamene anasinkhiwa na Mulungu kunkhala oweluzo bamoyo nabakufa.⁴³ Nikwayeve kwamene aneneri bonse apelekela umboni, kuti aliyense wamene akhulupilila muli yeve azalandila kukhululukiwa kwa macimo kupitila muzina yake.⁴⁴ Pamene Petro enze akali kukamba izi zinthu, Mzimu Oyela anagwela onse benzo mvelera ku uthenga wake.⁴⁵ Banthu bamene benze ku gulu ya mdulidwe ya okhulupilila -bonse baja banabwela na Petro -banadabwa, cifukwa mphaso ya Mzimu Oyela inathilidwa pali akunja.⁴⁶ Cifukwa banamvela aba bakunja kukamba vitundu vinangu noyamika Mulungu. Pamene apo Petro anayankha,⁴⁷ "Kansi kuli aliyense angalise manzi kuti aba banthu basabatizike, aba banthu bamene balandila Mzimu Oyela monga ise?"⁴⁸ Pamene apo analamulila kuti abatizike muzina la Yesu Kristu. Ndipo anamupempha kuti ankhale nabeve masiku yambili.

Chapter 11

¹ Manje ma apostoji na abale benzeli mu Yudeya banamvela kuti ba Kunja nabeve balandila mau ya Mulungu. ² Pamene Petro anabwela ku Yelusalemu, baja bamene benzeli ku gulu ya amudulidwe banamususha; ³ banakamba ati, unyanjana na banthu osadulidwa nakudya nabo!" ⁴ Koma Petro anayamba kubafotokozela nkhani yonse mufikapo; anakamba ati, ⁵ Nenzeli kupemphera ku tauni ya Yopa, ndipo nenzeli namaso mphenya pali contena ibwela pansi, monga cinyula cikulu kucokela kumwamba kubwela nama kona yake yali 4. Cinabwela kwa ine. ⁶ Ninayanganamo ndipo ninaganizilapo. Ninabona nyama zamendo yali 4 zili muziko, nyama zamusanga, nyama zokalaba pansi, na nyoni zamumwamba. ⁷ Ninamvera mau kukamba naine, "Myamuka, Petro; paya nakudya!" ⁸ Ninakamba ati, osati so, Lord: kulibe cosayela kapena codesedwa camene cinalowapo mukwamwa mwanga." ⁹ Koma mau yanayankha futi kucoka kumwamba, Camene Mulungu wayeleza, usaciitane codesedwa." ¹⁰ Ici cinacitika katatu, ndipo zonse zinabwelelamonso kumwamba. ¹¹ Ndipo apo onani, pamena apo panali bamuna batatu oyimilila pasogolo ya nyumba mwamene tenzelili; wanatumiwa kwa ine kucoka ku Sizeliya. ¹² Mzimu unanituma kuti niyende nabeve, ndipo kuti nisapusanise paki beve. Aba ba bale bali 6 banayenda naine, ndipo tinaloba munyumba ya uyu munthu. ¹³ Anatiuza mwamene anabonela mngelo kuyimilila mnyumba mwake nokamba ati, "Tuma amuna ku Yopa kuti babwelese Simoni ocedwa Petro. ¹⁴ Azakamba naiwe uthenga wamene uzapuluma nabo -iwe na nyumba yako yonse." ¹⁵ Pamene ninayamba kukamba nabeve, Mzimu Oyela unabwela pali beve, monga cenzeli kwa ife poyamba paja. ¹⁶ Ninakumbukila mau ya Ambuye, mwamene anakambila, "Yohane zoonadi anabatiza na mazi; koma muzabatizika mu Mzimu Oyela." ¹⁷ So ngati Mulungu anabapasa beve mphaso monga anatipasila pamene tinakhulupilila pali Ambuye Yesu Kristu, ndine ndani ine, kuti nitalikane na Mulungu?" ¹⁸ Pamene anamvera izi zinthu, palibe camene anakamba moyankha, koma anayamika Mulungu nokamba ati, "Kansi Mulungu wapasa kutembenuka kwa moyo kuli akunja nabeve." ¹⁹ Manje baja bamene banamwazikana cifukwa cakusausidwa kwamene kunayamba nopaiwa kwa Stefano banafika paka ku Fonisia, Saipulasi, naku Antioku, koma anakamba za uthenga wa Yesu cabe kuli ba Yuda. ²⁰ Koma benangu pali beve, bamuna ocokela ku Saipulasi na Sailini, anabwela ku Antioku nokambanso nama Giliki, kubauza za uthenga wabwino wa Ambuye Yesu. ²¹ Ndipo kwanja kwa Ambuye kwenzeli nabeve; namba ikulu maningi inakhulupilila notembenukila kwa Ambuye. ²² Uthenga pali beve unafika mumatu ya mpingo ku Yelusalemu: ndipo banatuma Banabasi kufika mpaka ku Antioku. ²³ Pamene anabwela nobona mphaso ya Mulungu, anakondwela, ndipo anabalimbikisa bonse kuti ankhale mwa Ambuye namtima wabo bonse. ²⁴ Cifukwa enzeli munthu wabwino nabozula na Mzimu Oyela, nacikhulupililo, ndipo banthu bambili banafakiliwako kwa Ambuye. ²⁵ Banabasi apo anayenda ku Tasisi kuyendo sakila Sauli. ²⁶ Pamene anamupeza, anamuleta ku Antioku. Cinabwela cacitika nicakuti, caka conse banasonkhana pamozi namupingo nophunzisa banthu bambili. Ophunzira banaitanidwa kuti Akristu koyamba ku Antioku. ²⁷ Manje pamasiku aya aneneri benangu banabwela kucoka ku Yelusalemu kubwela ku Antioku. ²⁸ Umozi mwa beve, Agabasi mwazina lake, anaimilila nobonesela mwa Mzimu kuti njala izacitika paziko lonse. Izi zinacitika mumasiku ya Kilaudiyasi. ²⁹ So, ophunzira, kulingana mwamene anakwanisila aliyense, anaganizila kutuma thandizo kuli abale ku Yudeya. ³⁰ Anacita ici; anatuma ndalama kuli akulu mumanja ya Banabasi na Sauli.

Chapter 12

¹ Manje pali iyo nthawi mfumu Herode anamanga bengu bamene anali bamumpingo kuti abasause. ² Anapaya Jemusi m'bale wake wa Yohane na lupanga. ³ Pamene anabona kuti ici cinakondwelesa Ayuda, anamanga futi Petro naye. Ayo yanali masiku yapwando la pasaka. ⁴ Pamene anamunga, anamuyika mujele anayika basilikali bali 4 mumagulu 4 kuti bamuyanganile yeve, ananganiza zomuleta kuli banthu pwando Yasaka itasila. ⁵ So Petelu anamusungila mujele, koma banamupempherera maningi kuli baja benzeli mumpingo. ⁶ Siku pamene Herode akalibe kumucosa, usiku uja Petro anagona pakati pa asilikali babili, omangidwa namacheni yabili, ndipo omuyanganila benzeli pasogolo paciseko benzo yanganila jele. ⁷ Onani apo, mngelo wa Ambuye anabonekela mwazizi pali yeve, ndipo laiti inabonekela mu celo. Anamugunduzza Petro pambali nomubusha nokamba ati, "Nyamuka mwamsanga." Ndipo ma cheni yake yanacoka mumanja mwake. Mngelo anakamba nayeve kuti, ⁸ "Zivalike wake ndipo vala namasanda. Petro anacita socabe. Mngelo anakamba nayeve ati, "Vala malaya yakunja ndipo unikonkhe." ⁹ So Petro anamukonkha ndipo anacoka. Sanazibe kuti camene cinacitika na mngero cenzeli ca zooni. Ananganiza kuti enzi ona maso mphenya. ¹⁰ Pamen anapita oyanganila oyamba nawacibili, anafika pageti yasimbi yamene yenzoyenda mu tauni; inazisegukila yeka kuli beve. Banacoka ndipo banayenda mumsebo, ndipo pamene apo mngero anamusiya yeka. ¹¹ Pamene Petro anazindikila zamene zinacitika, anakamba ati, "Manje niziba kuti Ambuye atumu mngero wabo kunicosa mumanja ya Herode, nakuciyembezo ca banthu aci Yuda." ¹² Pamene anazindikila izi, anayenda kunyumba ya Maria maiwake wa Yohane wamene ciwongo cake ni Mariko; okhulupilila bambili benzeli banakumana kwamene ndipo benzopemphera. ¹³ Pamene anagogoda paciseko ca gedi, wanchito mkazi zina lake Roda anayankha. ¹⁴ Pamene anazindikila mau ya Petro, mwacimwemwe anakangiwa kusegula ciseko; m'malo mwake anabwela anathamangila mucipinda; norepota kuti Petro enzeli imilile paciseko. ¹⁵ Ndipo anakamba kuti kwa yeve, "Ndiwe ofuntha." Koma analimbikila kuti ndiye mwamene cilili. Banabwela bakamba ati, "Nimungelo wake." ¹⁶ Koma Petro anapitiliza kugogoda, ndipo pamene anasegula ciseko, banamuona ndipo anadabwa. ¹⁷ Petro anabakambisa nakwanja kwake kuti bankhale zii, ndipo anabauza mwamne Ambuye banamucosela mujele. Anakamba ati, Muripote ivi vinthu kuli Jemusi na abale." Ndipo anacoka noyenda kumalo yenangu. ¹⁸ Manje pamene kunaca, kwenzelibe cisangalaro ciliconse pakati pa asilikali, pazamene zinacitika pali Petro. ¹⁹ Pamene Herode anamusakile yeve ndipo sanamupeze, anafunsa oyanganila ndipo anapeleka lamulo kuti apayiwe. Ndipo anacoka ku Yudeya noyenda ku Sizeliya nonkhala kwamene kuja. ²⁰ Manje Herode enzeli okalipa nabanthu baku Taila na Sidoni. Banayenda kuli yeve pamozi. Banagonjesa Bulatasi, othandizila mfumu, kuti abathandize. Anapempha mtendere, cifukwa ziko lao inlandila vakudya kucoka ku ziko la mfumu. ²¹ Pasiku yoikika Herode anazivalika zovala va ufumu nonkhala pamu pando wacifumu, anapeleka mau kwa beve. ²² Banthu banapunda ati, "Aya nimau yakamulungu, osati yamunthu!" ²³ Pamene apo mngero wa Ambuye anachaya yeve, cifukwa sanapase Mulungu ulemelero; anadyewa nanyongolosi nomwalila. ²⁴ Koma mau ya Mulungu yanafalikila nopakilako. ²⁵ Pamene Banabasi na Sauli anasiliza nchito yao ku Yelusalemu, banacokako uko; banatenga Yohane wamene ciongo cake ni Mariko. (Ma baibolo yene yebelenga kuti, Banabasi na Sauolo anabwelela ku Yelusalemu (olo kuja))

Chapter 13

¹ Manje mpingo waku Antioku, mwenzela ma aneneri na aziphunzisi. Benzeli Banabasi, Simiyoni (oyitanidwa Niga, Lusiyasi waku Sailini, Maniyani (muzake wa Herode), na Sauli. ² Pamene benzeli kutamanda Mulungu nosala kudya, Mzimu Oyela anakamba ati, "munipatulile Banabasi na Sauli, kuti bacite nchito yamene nabaitanila." ³ Pamene banasiliza kusala kudya, nopephela, nobafaka manja yabo pali aba bamuna, banacoka. ⁴ So Banabasi na Sauli banamvelera Mzimu Oyela ndipo banayenda ku Seleusia; kucoka kuja banakwela boti noyenda kumalo ya Siprasi. ⁵ Pamene benzeli mu tauni ya Salamisi, banalalikila mau ya Mulungu mumasinagoge ya Ayuda. Benzelinso na Yohane Mariko monga obathandiza. ⁶ Pamene banayenda pamala ponse pa Pafosi, anapeza wamajiki winangu, mneneri waboza Waciyuda, wamene zina lake ni Bar Yesu. ⁷ Uyu wamajiki anagwilizana na govana, Segiayasi Paulusi, wamene enzeli mwamuna wa nzelu. Uyu munthu anaitana Banabasi na Sauli, cifukwa enzo funa kumvera mau ya Mulungu. ⁸ Koma Elimasi "wamajiki" (ndiye mwamene zina lake imasulilidwa) anabasusha; anayesesa kuosa govana kucoka kucikhulupiliro. ⁹ Koma Saulo, wemenenso ezoitaniwa kuti Paulo, ozazidwa na Mzimu Oyela, anamuyanganisisa maningi nokamba ati, ¹⁰ "Iwe mwana wa Satana, ndiwe ozula na maboza yonse nakuipa. Ndiwe mudani paciliconse cabwino. Suzakwanisa kubendesa njila za straiti za Ambuye, kansi uzacita so?" ¹¹ Manje ona, kwanja kwa Mulungu kuli paiwe, ndipo uzankhala ulibe menso. Suzaona zuba pakanthawi." Pamene apo panagwela pali Elimasi vambuu namudima; anayamba kuyenda yenda kupempha banthu kuti bamugwile pa kwanja nomusogolela. ¹² Pamene govana anawona vamene vinacitika, anakhulupilila, cifukwa anadabwa pali vipfunziso pali Ambuye. ¹³ Manje Paulo nabazake banayenda ku Pafosi nofika ku Pega ku Pafilia. Koma Yohane anabasiya nobwela ku Yelusalemu. ¹⁴ Paulo nabazake anayenda kucoka ku Pega noyenda ku Antioku ku Pisidiya. Kuja banayenda mumasinagoge pa Sabata ndipo anankhala pansi. ¹⁵ Pamene banabelenga lamulo naba neneri, asogoleli bamusenagoge anabatumila uthenga kukamba kuti, "Abale, ngati muli nauthenga olimbikisa aba banthu, ukambeni. ¹⁶ So Paulo ananyamuka nonyamula kwanja; nokamba ati, "Bamuna baku Israyeli naimwe bamene mulemekeza Mulungu, mverani. ¹⁷ Mulungu wa aba banthu waku Israyeli anasankha azitate bathu nopanga banthu kupaka pamene banankhala mumalo ya Egypto, Nakwanja kwamphamvu anabacosamo. ¹⁸ Kwazaka ngati 40 anabalekela mucipululu. (Ma baibulo yenengu yebelenga kuti, ko kwanila zaka 40 anabasamalila mu cipululu.) ¹⁹ Pamene anabononga vialo vili 7 mu malo ya Kenani, anapasa banthu bathu malo yabo kunkhala yabo. ²⁰ Vonse ivi vocitika vanacitika pazaka zili 450. Pamene vinasila ivi vonse, Mulungu anabapasa oweluzi mpaka Samuyeli muneneri. ²¹ Banthu panapempha kuti abapase mfumu, ndipo Mulungu anabapasa Sauli mwana wa Kishi, mwamuna ocokela ku banja ya Benjamini, kuti ankhale mfumu zaka zokwanila 40. ²² Pamene Mulungu anamucosa pa ufumu, ananyamula Davide kuti ankahale mfumu. Cenzeli pali Davide pamene Mulungu anakamaba, 'Napeza Davide mwana wa Jeseckunkhala mwamuna wapa mtima panga, wamene acita vilivonse vamene nifuna iye acita.' ²³ Kucoka kumubado wauyu munthu Mulungu waleta kwa Israyeli mphulumusi, Yesu, monga mwamene analonjezela. ²⁴ Ivi vanayamba kucitika pamene, Yesu sanabwele, Coyambilila Yohane ananounsa upatizo wotembenuka ku wanthu onse waku Israyeli. ²⁵ Pamene Yohane enzasiliza nchito yake, anakamba ati, 'Kodi munganiza kuti ndine ndani? Sindine wamene. Koma mvesesani, kuliwina abwela pasogolo panga, wamene nthambo za sapato zake sindine oyenela kuzimasula.' ²⁶ Abale, bana ocoka kuli Abrahamu, naimwe pakati panu wamene mulambila Mulungu, sikwaise kuti mau yacipulumuso yatumidwa. ²⁷ Kwa iwo wamene ankhala mu Yelusalemu, nabolamulila bawo, sibanamuzindikile iye, ndipo wanakwanilisa zokambika za aneneri zamene zibelengedwa sabata iliyonse pakumuweluzi iye. ²⁸ Ngankhale kuti sibana peze cifukwa cenini comupaila iye, anauza Pilato kuti amupaye. ²⁹ Pamene banasiliza zinthu zonse zamene zinalembedwa za yeve, banamucosa mumtengo nomushika mumanda. ³⁰ Koma Mulungu anamuusha kuli wakufa. ³¹ Banamuona masiku ambili nawaja bamene wanabwela nayeve kucoka ku Galileya kubwela ku Yelusalemu. ³² So tibwelesa uthenga wabwino pamalonjezo yanapangiwa kuli azitate bathu: ³³ Mulungu anasunga aya malonjezo kwa ise, kubana bawo, kuti anausha Yesu kubwelesa kumoyo. Izi ndiye zamene zinalembedwa muma Salimo wacibili: 'Ndiwe mwana wanga, lero nankhala Tate wako.' ³⁴ Pali zoonza kuti anamuusha kwa kufa kuti thupi yake sizabwele mkubola, akamba socabe: 'Nizakupasani zoyela namadaliso yene ya Davide.' ³⁵ Nicifukwa cake akamba futi muma Salimo inangu, 'Suzalola Oyela wako kuti abole.' ³⁶ Pamene Davide apanga mubado wake kutumikila zenzo funa Mulungu, anagona (anamwalila), noshikiwa na azitate bake, ndipo anabola, ³⁷ koma iye wamene Mulungu anausha sanabole. ³⁸ So lekani cizibika kwa inu, abale, kupitila muli uyu munthu kulalikidwa kukhululukidwa kwa macimo. ³⁹ Kupitila mwa iye aliyense wakhulupilila alungamisiwa kuzithu zonse zamene lamulo ya Mose sinakwanise kulungamisa. ⁴⁰ So cenjelani kuti zinthu zamene aneneri anakambapo siziza ciktika kwa imwe: ⁴¹ 'Onani, imwe opepusa, mudabwisike ndipo mubonongeke; cifukwa nicita nchito mumasiku yanu, Nchito yamene

simuzaikhulupilila, ngakhale kuti winangu ayinaunsa kuli imwe."⁴² Pamene Paulo na Banabasi wenzocoka, banthu anabapempha kuti baka kambe futi aya mau yamozi nayamozi sabata yamene ibwela.⁴³ Pamene musonkhano wamusinagoge unasila, Ayuda bambili nabaja ozipeleka kuciyuda anakonkha Paulo na Banabasi, banakmba nawo nobalimbikisa kuti apitiliza mucisomo ca Mulungu.⁴⁴ Sabata yokonkhapo, pafufupi tauni yonse banakumana pamozi kuti bamverele mau ya Ambuye.⁴⁵ Pamene Ayuda anabona gulupu, banamvela jelasi noyamba kukamba mosushana navamene enzo kamba Paulo nomunyoza.⁴⁶ Koma Paulo na Banabasi anakamba mwaphamvu nokamba ati, "Cenzeli cofunikila kuti mau ya Mulungu ya yambilile kulalikilidwa kuli imwe. Kuona kuti muyapushing'a kutali kuli imwe ndipo muziyesa osayenela ku umoyo osatha, onani, tizayenda kuli Akunja.⁴⁷ Cifukwa Ambuye atilamulila, kunena kuti, 'Nakuikani kunkhala nyali kwa Akunja, kuti mupeleke cipulumuso kumalekezelo yonse ya calo.'" ⁴⁸ Pamene Akunja banamvera izi, banakondwela noyamikila mau ya Ambuye. Pabambili bamene anasankhidwa ku umuyo osatha banakhulupilila.⁴⁹ Mau ya Ambuye yanaperekewa ponse ponse mumzida onse.⁵⁰ Koma Ayuda analimbikisa azimai ozipeleka naboyenela, nabamuna benze osogolela mutauni. Banapangisa kusausidwa kwa Paulo na Banabasi nobaponya kupitilila kunja kwa tauni.⁵¹ Koma Paulo na Banabasi anabana kukhumula kalukungu kucoka kumendo yabo. Pamene apo anayenda ku Tauni ya Ikoniya.⁵² Ndipo ophunzila anambela cimwemwe nozuzhiwa na Mzimu Oyela.

Chapter 14

¹ Cinacitika mu Ikoniya mu kuto pame Paulo na Banabasi alowa pamozi mu sinagoge ya Ayuda nokamba munjila yakuti banthu bambili Ayuda na Acigiliki anakhulupilila. ² Koma Ayuda amene senzomverela anapangisa manganizo ya Akunja kunkhala okalipa pali abale. ³ So banankhala kuja nthawi itali, kukamba mwamphamvu namphamvu ya Ambuye, pamene enzo peleka umboni pali uthenga wacisomo. Anacita ici pakusa visanzo navodabwisa vingacitika kupitila mu manja ya Paulo na Banabasi. ⁴ Koma bambii mu tauni banagabikana: benengu banthu banankhala kusaidi ya Ayuda, benangu kusaidi yama apostozi. ⁵ Pamene Akunja pamozi na Ayuda anayesa kukoka asogoleli bawo kuti basause notema myala Paulo na Banabasi, ⁶ banabwela baziba pali ici nothabila kuma tauni ya Likoniya, Lisitila naDebi, namizinda yozungulila, ⁷ ndipo kuja benzo lalikila uthenga. ⁸ Ku Lisitila mwamuna winangu anankhala, alibe mphamvu pamendo pake, olemala kucoka mumala ya amai bake, sanayendepo. ⁹ Uyu munthu anamvera Paulo ali kukamba. Paulo anaika menso yake pali yevenobwelo uwona kuti ali nacikhulupililo kuti angankhale bwino. ¹⁰ So anakamba nayeve mopunda, "Nyamuka." Ndipo uja mwamuna anajumpha noyamba yenda yenda. ¹¹ Pamene gulu inaona vamene anacita Paulo, anakweza mau yawo, kukamba mucithundu caku Likoniya, "Milungu yabwela kwa ise mukupitila mu banthu." ¹² Banaitana Banabasi kuti "Ziyasi," na Paulo, kuti "Hemasi," cifukwa enzeli mwine wokamba. ¹³ Wa sembe wa Ziyasi, wamene tempele yake inali panja pa tauni, analeta ng'ombe namaluba pageti; yeve nagulupu benzofuna kupeleka nsembe. ¹⁴ Koma pamene ma apostozi, na Banabasi na Paulo, anamvera za ici, banang'amba malaya yawo ndipo mwamsanga banayenda pagulu, kulila ¹⁵ nokamba kuti, Bamuna imwe, nicifukwa nicani mucita ivi vinthu? Ise nase ndise banthu nazomvera monga zanu. Tikubwelesalena uthenga wambwino, kuti mucoke kuli ivi vinthu vilembe nchito nobwela kuli Mulungu wamoyo, wamene anapanga kumwamba, na ziko lapansi, namimana navonse vamene vilimo. ¹⁶ Kumbuyo uku, anavomeleza vialo vonse kuyenda munjila zawo. ¹⁷ Koma apo, sanazisiye yeka kunkhala alibe umboni, cifukwa cakuti anacita bwino nopasa imwe mvula kucoka kumwamba nanyengo zocita bwino, kukwanilisa mitima yanu navakudya nacimwemwe." ¹⁸ Ngankhale na mau aya, Paulo na Banabasi sanakwanise kulesa gulu kupeleka nsembe kuli beve. ¹⁹ Koma Ayuda benangu ocokela ku Antioku na Ikoniya mu anbwela kugonjesa gulupu. Banamutema myala Paulo nomucosa mu tauni, kuganizila kuti anafa. ²⁰ Koma pamene aphunzila benze anaimilila kuzungulila yeve, ananyamuka noloba mu tauni. Siku yokonkhapo, anayenda ku Debi pamozi na Banabasi. ²¹ Pamene banalalikila uthenga mu tauni muja nopanga ophunzila ambili, banabwelela ku Lisitira, paka ku Ikoniya na Antioku. ²² Anapitiliza kulimbikisa moyo wa ophunzila nobalimbikisa kuti apitilize mucikhulupililo, kukamba kuti, "Tifunika kuloba mu Ufumu wa Mulungu kupitila muma sauso yambili." ²³ Pamene banaba sankhila akulu ampingo mumpingo ulibonse, ndipo anapemphela nosala kudya, anabapeleka kwa Ambuye, mwa iye wamene anakhulupilila. ²⁴ Ndipo apo anapitila mu Pisidiya nobwela ufika ku Pafaliya. ²⁵ Pamene banalalikila mau mu Pega, banayenda ku Attaliya. ²⁶ Kucoka uko banayenda ku Antioku, kwamene benzeli ozipoleka ku cisomo ca Mulungu pa nchito yamene manje banasiliza. ²⁷ Pamene banafika mu Antioku nobwelesa mpingo pamozi, banarepota vinthu vonse vamene Mulungu anacita pamozi nabeve, namwamene anasegulila njila yacikhulupililo kuli bakunja. ²⁸ Banankhala thawi itali nawophunzila.

Chapter 15

¹ Bamuna benangu banacoka ku Yudeya nomphunzisa abale, kunenakuti, pokhapo mukadulidwa monga pa mwambo wa Mose, simungapulumusidwe." ² Pamene Paulo na Banabasi anakangana nocita nawo ndale, abale anaganiza kuti Paulo, Banabasi nabena afunika kuyenda ku Yelusalemu kuli ma apostozi na akulu pali iye nkhani. ³ Ndipo apo, pakutumidwa nampingo, anapitila ku Fonisiya na Samaria nocita anaousi kutembenuka kwa Akunja. Anabwelesa cisangalalo cacikulu kuli abale onse. ⁴ Pamene anafika ku Yelusalemu, analandliwa na mpingo nama apostozi na akulu, ndipo analipota zonse zinthu zamene Mulungu anacita pamozi naiwo. ⁵ Koma amuna bena bamene anakhulupilila, enzeli ku gulupu ya Afalisi, anaimila nokamba ati, "nicofunikila kubacita mdulidwe nakubalamulila kuti asunge malamo ya Mose. ⁶ So ma apostozi na akulu anakuma pamozi kuti ayanganepo iyi nkhani. ⁷ Pamene banakambilana kwa nthawi itali, Petulo ananyamuka nokamba kwa iwo, "Abale, muziba kuti panthawi yambwino yamene yapita Mulungu anasankha pakati pawo, kuti kupitila mukamwa mwanga Akunja amvele mau awuthenga, nokhulupilila. ⁸ Mulungu, aziba mtima, abapasa umboni, kubapasa Mzimu Oyela, monga mwamene anacitila ise; ⁹ ndipo sanapange kupatula pakati pa ise nabeve, kupanga mitima kuyela mwacikhulupililo. ¹⁰ Mwanje nicifukw ninji muyesa Mulungu, kuti muyike joko pamikosi yaophunzila yamene ngakhale azitate bathu kapena banakwanisa kucilandila? ¹¹ Koma tikhulupilila kuti tizapulumusika kupitila mcisomo ca Ambuye Yesu, monga cinalili kwabeve." ¹² Gulu yonse inankhala zii pamene benzomvela Banabasi na Paulo penzo repota pa visanzo na vodabwisa Mulungu anacita pakati pa Akunja kupyolela mwabeve. ¹³ Pamene banaleka kukamba, Jemusi anayankha, nokamba ati, Abale, mvelani kwa ine. ¹⁴ Simoni wakamba mwamene Mulungu poyamba mwacisomo anathandizila Akunja kuti mwabeve atenge banthu kwa zina lake. ¹⁵ Mau y aneneri yanagwilizana nazeve, monga kunalembewa, ¹⁶ 'Zikasila izi zinthu nizabwelela, Ndipo nizamanganso tenti ya Davide, yamene inagwa; Nizainyamula noibwezelo, ¹⁷ kuti baja bamuna banasala akafune Ambuye, kuyikilako akunja oyitanidwa na zina langa. ¹⁸ Ici ndiye camene Ambuye akamba, nindani wacita izi zinthu zamene zinazibika kucoka kudala. (Ma Baibulo inangu yabelenga guti, Ici ndiye camene Ambuye akamba, kwamene zizibika zonse zocitita zake kucoka kudala.) ¹⁹ Cifukwa ca ici, maganizo yanga ni aya, kuti tisavutise baja acikunja bamene babwela kwa Mulungu; ²⁰ koma kuti tibalembele kuti bacoke kupemphelera mafano, kuciwelewele, nacakufa ceka, namwazi. ²¹ Kucoka ku mibado yakudala kulibanthu mu tauni iliyonse bamene alalikila nobelenga Mose mumasinagoge sabata ili yonse." ²² Ndipo cinaboneka bwino kuli ma apostozi na akulu, namupingo bonse, kusankha Yudas oyitanidwa Basabasi, na Sailasi, amene anali azisogoleli mu mpingo, nobatuma ku Antioku pamozi na Paulo na Banabasi. ²³ Analemba izi: "Ma apostozi, akulu na abale, kwaAkunja abale ku Antioku, Siriya na Cilisiya, moni. ²⁴ Tinamvela kuti ba muna benangu bamene tinapasa malamulo maningi, banacoka kuli ise ndipo bakuvutisani naviphunziso vamene vivutisa moyo yanu. ²⁵ So cinatibonekela bwino tonse kuti tigwilizane kuti tisankhe banthu nobatuma kwa imwe okondedwa Banabasi na Paulo, ²⁶ banthu bamene baika moyo wabo pangosi cifukwa ca zina la Ambuye Yesu Kristu. ²⁷ Tuma cifukwa caici Yudas na Sailasi, bamene azakuuzani zinthu zimozi nazimozi. ²⁸ Cifukwa cinaoneka bwino kwa Mzimu Oyela na kwa ise, kuika paimwe katuntdu olema kupambana izi zinthu zofunikila: ²⁹ kuti mucoke ku vinthu vopelekewa nsembe kumafno, mwazi, vakufa veka, nakuciwele wele. Ngati muzisunga kuli ivi vinthu, zizankhala bwino na imwe. Mukhale bwino." ³⁰ Ndipo beve, pamene banamasulidwa, anabwela ku Antioku; anabwelesa banthu pamozi, anapeleka kalata. ³¹ Pamene anaibelenga, banakondwela cifukwa ca cilimbikiso. ³² Yudas na Sailasi, na neneri, analimbikisa abale namau ambili nobalimbikisa. ³³ Pamene banankhalako pakanthawi, banabamasula mwamutendele kucoka ku abale kuli beve bamene anabatuma. ³⁴ (Koma cinamuonekela bwino Sailasi kusalila). ³⁵ Koma Paulo na Banabsi anankhala mu Antioku pamozi na bene bambili, kwamene anaphunzisa nolalikila mau ya Ambuya. ³⁶ Pamene panapita nthawi Paulo anakamba ati kwa Banabsi, "Tiye tibwelele manje tikayendela abale mutauni iliyonse kwamene tinalalikila mau ya Ambuye, nobona mwamene alili. ³⁷ Banabasi anafunanso kuti atenge Yohane woitanidwa Mariko. ³⁸ Koma Paulo anaganiza kuti sicinali cabwino kutenga Mariko, wamene anabasiya ku Pafaliya ndipo sanapitilize nchito pamozi nayeve. ³⁹ Ndipo kunapezeka kusushana kwambili, kufika mpaka banapatukana, ndipo Banabasi anatenga Mariko noyenda ku Sipulasi. ⁴⁰ Koma Paulo anasankha Silasi ndipo anacoka, pambuyo pobapasa kuti asalalile mwacisomo ca Ambuye. ⁴¹ Ndipo anapitila ku Siliya na Silisiya, kulimbikisa mipingo.

Chapter 16

¹ Paulo anabwelanso ku Debi na Lisitila; ndipo onani, ophunzira wina zina lake Timoteyo analiko, mwana wa mzimai waci Yuda wamene anali okhulupilila; atate bake enzeli waci Giliki. ² Banakamba zambino za iye abale bamene anali ku Lisitira na Ikoniya. ³ Paulo anamufuna kuti ayende naye; so anamutenga iye nomucita mudulidwe cifukwa ca Ayuda amene anali kumalo ayo, cifukwa bonse banaziba kuti atate bake benzeli ba Giliki. ⁴ Pamene benzo kupitila mu matauni, banapeleka ku mipingo malamulo kuti iwo amverele, malamulo yamene yanalembedwa nama apostoji na akulu mu Yelusalemu. ⁵ So mipingo inalimbikisika mucikhulupililo nopakilapo munamba sikuku nasiku. ⁶ Paulo nabanzake banayenda kupitila mumizinda ya Flagiya na Galatiya, cifukwa Mzimu Oyela anabalesa kulalilikila mau ku mizinda ya Azia. ⁷ Pamene banafika pafupi na Masiya, anayesa kuyenda ku Bitaniya, koma Mzimu wa Yesu onabalesa. ⁸ So popitila ku Masiya, anafika kutauni ya Traosi. ⁹ Masophenya yanamuonekela Paulo usiku: mwamuna waku Masedoniya anali imilile paja, kumuitana nokamba ati, Bwela kuno ku Masedoniya utithandizile. ¹⁰ Pamene Paulo anabona masophenya, pamene apo tinayenda ku Masedoniya, kuganizila kuti Mulungu anabaitana iwo kuyendo lalikila uthenga kwa beve. ¹¹ Kunyamuka kucoka ku Traosi, tinanyamuka kuyenda ku Samoterace, ndipo siku yokonkhapo tinayenda ku Niyapolisi; ¹² kucoka uko tinayenda ku Filipi, yamene ni tauni ya Masedoniya, tauni yofunikila maningi mu boma na mu Roma, ndipo tinankhala mu tauni iyi masiku yambili. ¹³ Pa Sabata tinayenda panja pa geti kumbali kwa mumana, kwamene tinaganiza kuti kuli malo yopemphelerako. Tinankhala pansi nokamba na azimai bamene enze anabwela pamozi. ¹⁴ Mkazi winangu ocedwa Lidiya, ogulisa va pepo kucoka ku tauni ya Tiya-tira, wamene anapembeza Mulungu, anativelela. Ambuye anasegula mtima wake kumverele kuvamene Paulo anakamba. ¹⁵ Pamene anabatizika, nanyumba, anatilimbikisa, nakukamba kuti, "ngati mwaniweluzi kunkhala okhulupililika kwa Ambuye, bwelani kunyumba kwanga, nonkhala naine." Ndipo atigonjesa. ¹⁶ Cinabwela cacitika kuti, pamene tenzoyenda kumalo yopemphelerako, msikana winangu wamene enzeli namuzimu olota anakumana nase. Anapangila abosi bake ndalama zambili muzokamba zake. ¹⁷ Uyu msika anakonkha Paulo na ise nopunda, kukamba ati, "Aba banthu nibanchito ba Mulungu Mkulu kulu. Balalikila kwa imwe njila ya cipulumuso. ¹⁸ Anacita ici masiku yambili. Koma Paulo, pamene anakalipa maningi naive, anapindimuka nokamba kwa mizimu, Nikulamulila muzina la Yesu Kristu kuti ucoka mwa yeve." Ndipom cinacoka pamene apo. ¹⁹ Pamene ba bosi bake anabona kuti popangila ndalama payenda, banamumanga Paulo na Sailai nobapeleka pamaketi pamenso yaolamulila. ²⁰ Pamene anabaleta kuli oweluza, anakamba ati, "aba banthu na Yuda ndipo bapanga mambuto yambili mu tauni mwathu. ²¹ Baphunzisa zinthu zosalolelwa kuti ise tilandile or kulondola ngati Aroma." ²² Ndipo gulu inanyamukila pamozi ku ukila Paulo na Sailasi; oweluza banang'amba malaya yabo nakubavula nolamulila kuti bamenyedwa nandodo. ²³ Pamene banabamenya maningi, banabaponya mundende nolamulila wogading'a kuti abafakeko nzeru maningi. ²⁴ Pamene analandila lamulo iyi, wogading'a anabaponya mukati maningi mwa jele nomanga mendo yawo maningi. ²⁵ Pakati pa usiku Paulo na Sailasi benzo pemphela noyimba nyimbo kwa Mulungu, ndipo bakaidi benangu benzo bamvelerela. ²⁶ Mwazizi kwenzeli kung'ambika pansi kukulu, mpaka maziko yamujele yanagwendezeka; ndipo pamene apo viseko vinaseguka, ndipo macheni ya aliyense yanamasuka. ²⁷ Wogading'a anauka patulo nowona kuti viseko vamujele nivoseguka; anacosa cinayifi cake nonkhala pang'ono kuzipaya, cifukwa anaganiza kuti bakaidi bathaba. ²⁸ Koma Paulo anapunda maningi, kukamba kuti, osazipanga ngozi, cifukwa tonse tilimo muno." ²⁹ Wogading'a anaitanisa laiti nobwelo ngena, nishi anjenjema namantha, nokugwa pansi pali Paulo na Sailasi, ³⁰ nobacosa panja nobwelo akamba ati, Kansi ningacite bwanji kuti nipulumuke?" ³¹ Banakamba ati, Khulupilila mwa Ambuye Yesu, ndipo uzapulumusika, iwe na banja lako lonse. ³² Banakamba mau ya Ambuye kwa yeve, pamozi nabonse benzeli munyumba mwake. ³³ Pamene apo gadi anabatenga pa nthawi yamene iyo yausiku, nobasanbika mendo vilonda vabo, ndipo yeve nabanja lake lonse anabatizika pamene apo. ³⁴ Anabwelesa Paulo na Sailasi kunyumba kwake nobapasa vakudya. Anasangala maningi nanyumba yake yonse, cifukwa bonse anakhulupilila Mulungu. ³⁵ Pamanje pamene kwenzeli muzuba, oweluza anatuma mau kuli magadi nokamba ati, Leka abo banthu bayende." ³⁶ Gadi anarepota mau kwa Paulo, kukamba ati, "Oweluzi anituma mau kuli ine kuti nibamasule: manje so cokani, muyende bwino. ³⁷ Koma Paulo anakamba ati kuli beve, "Banatimenya pacigulu, banthu balibe mulandu aci Roma, ndipo mwatifaka mujele; manje apa bafuna baticose mwaci sini? Yai ndithu, balekeni babwele beka kuti baticose. ³⁸ Magadi anapeleka aya mau kuli oweluza; oweluza anamvera mantha pamene banmvera kuti Paulo na Sailasi benzeli ba Roma. ³⁹ Oweluza anabwela kubapapata; ndipo pamene anabacosa mukele, anauza Paulo na Sailasi kuti acoke mu tauni. ⁴⁰ So Paulo na Sailasi anacoka mujele noyenda kunyumba kwa Lidiya. Pamene Paulo na Sailasi anabona abale, anabalimbikisa ndipo banacoka mu Tauni.

Chapter 17

¹ Manje pmene banapita mumatauni ya Amfipolisi na Apoloniya, banafika ku tauni ya Thesalonika, kwamene kwenzeli sinagoge ya Ayuda. ² Paulo, monga pa mwambo wake, anayenda kwa yeve, ndipo pa masiku yali 3 ya Sabata anabamasulila malemba. ³ Enzo sengula malemba nofotokoza kwa beve kuti cenzeli cofunikila kwa Kristu kubvutika ndiponso ku ukanso kwa bakufa. Anakamba kuti, Uyu Yesu wamene nilalikila kwa imwe ndiye Kristu." ⁴ Benangu ba Yuda banakhulupilila ndipo banajoina Paulo na Sailasi, kufakila ma Giliki ozipeleka, nabazimai osogolela nagulupu ikulu. ⁵ Koma baYuda bamene sibanakhulupilile, pakunkhala na jelasi, anatenga bazibambo banangu oipa bapamaketi, noleta gulu pamozi, notufya banthu mu tauni kuti bapange viongo. Pakubononga nyumba ya Jasoni, banafuna kuleta Paulo na Sailasi pabanthu. ⁶ Koma pamene sanabapeze, banadosa Jasoni nabenangu ba bale pamenso ya bakulu bakulu bamutani ninshi, balila kuti, ⁷ "Aba bazibambo bamene basokoneza calo wabwela kuno futi. Aba bazibambo bamene Jasoni walandila bacita mosushana nalamulo ya Siza; bakamba kuti kuli mfumu inangu -Yesu." ⁸ Pamene gulu naba kulu bakulu ba tauni banamvela izi zinthu, benzeli mumabvuto. ⁹ Pamene banatenga ndalama kuli Jasoni nabinangu, anabatailila. ¹⁰ Usiku uja bale banatuma Paulo na Sailasi ku Beriya. Pamene banafika kuja, banayenda ku sinagoge ya Yuda. ¹¹ Manje aba banthu benzeko bwino kupambana baja baku Thesalonika, cifukwa banalandila mau namanganizo yokonzekela, kusanthula malemba kuti babone ngati izi zinthu zili mwamene zilili. ¹² Cifukwa caici bambili banakhulupilila, kufakilapo nabazimai baci Giliki na azibambo bambili. ¹³ Koma pamene Ayuda baku Thesalonika banamvela kuti Paulo analinso kulalikila mau ya Mulungu ku Beriya, banayendako noleta viongo nobvuta gulu. ¹⁴ Ndipo pamene apo, abale banatuma Paulo ayende kucimuna, koma Sailasi na Timoteyo banankala kwamene kuja. ¹⁵ Baja bamene benzo sogolela Paulo banamupeleka paka ku tauni ya Athenzi. Pamene banamusiya Paulo kuja, banalandila vofunika kucita va Sailasi na Timoteyo kuti wabwele msanga kwa yeve monga cili cofunikila. ¹⁶ Manje pamene Paulo enzo bayembekezela ku Athenzi, mzimu wake unabvutika pamene anaona kuti tauni yenzeli yozula namafano. ¹⁷ So anakambilana mu sinagoge naba Yuda nabonse benzo lambila Mulungu nabonse bamene benzo kumana nabo siku na siku pamalo yamaketi. ¹⁸ Komanso anakumana nabengu baku Ipiquliyani nabaja bokamba kuti chalo cinapangiwa mwa chansi. Ndipo benangu banakamba ati, kansi uyu okamba-kamba afuna kukamba cani?" Benangu banakamba ati, "Aboneka ngati nimulaliki watumilungu twacilwendo," cifukwa enzo lalikila pali Yesu naku ukisidwa. ¹⁹ Banamutenga Paulo nomuleta kuli Ayelopagasi, nokamba kuti, Tifuna tizibe ici ciphunziso cacilwendo camene wenzo kambapo? ²⁰ Cifukwa uleta zinthu zacilwendo mumatu yathu. Cifukwa caici, tifuna tizibe tanthauzo ya izi zinthu." ²¹ (Manje bonse ma Atheniyanzi nabalendo bonkhala muja bana sebenzesa nthawi yawo mukukamba kapena kumvelela cinthu cinangu ca manje.) ²² So Paulo anaimilila pakati pali Ayelopagasi nobwelokamba ati, "Imwe bamuna baku Athenzi, nawona kuti ndiwe bacipembezo munjila iliyonse. ²³ Cifukwa pamene nenzo pita nowona kuti zinthu zacyyamiko zanu, napeza guwa yolembewa kuti, "Kwa Mulungu osazibika." Pacamene mulambila mosaziba, ici cebve ninaunsa kwa imwe. ²⁴ Mulungu wamene anapanga calo navonse vilimo, cifukwa ni Ambuye wa kumwamba nacalo capansi, sankhala mumatempete yopangiwa namanja. ²⁵ Kapena kutumikiliwa namanja yabanthu, monga ngati enzofuna kalikonse, cifukwa cakuti yebve apasa banthu umoyo namphopo nazonse cabe. ²⁶ Ndipo kucokela kumunthu umozi anapanga ziko iliyonse yabanthu bamene bankhala pano pacalo capansi, pakubapangila nyengo yawo yo ikika nomolekezela ponkhala pawo. ²⁷ Cifukwa ca ici afunika kusakila Mulungu, ndipo mwina bangamufike yebve nomupeza, ndipo zoonza, salipatali kuli aliyense wa ise. ²⁸ Cifukwa mwa yeve tiyenda nonkhala na moyo, monga winangu mwaimwe alina ndakatulo wakamba kuti, 'Naise futi ndise bana bake.' ²⁹ So, cifukwa cakuti ndise bana ba Mulungu, sitifunika kuganiza kuti umulungu uli ngati golide, olo siliva, olo miyala, yosemedwa nabosema kapena maganizo ya munthu. ³⁰ Cifukwa ca ici Mulungu analekelela nthawi yakusaziba, koma manje alamulila banthu bonse kulikonse kuti atembenuke. ³¹ Ici nicifukwa baika sikupamene azaweluza calo mucilungamo mwabanthu bamene anasankha. Mulungu anapasa pulufu pali uyu mmwamuna kuli aliyense pakumuusha kwa akufa." ³² Manje pamene bamuna baku Athenzi banamvera za kuuka kwa akufa, benangu banamuseka Paulo; koma binangu banakamba ati, Tizakakumverela futi pali iyinkhani." ³³ Pambuyo pake, Paulo anayenda. ³⁴ Koma banthu benangu banamujoina nomukhulupilila, kufakilapo Dionishasi oweluza, nabenangu benzeli nawo.

Chapter 18

¹ Pamene vinasila ivi Paulo anacoka mu Athenzi noyenda ku Korinto. ² Kuja anapeza mu Yuda winangu zina lake ni Akwila, mwamuna waku Pontasi pamutundu; enza anacoka ku Itali camanje manje pamozi namukazi wake Prisila, cifukwa Kilaudi analamulila kuti bonse Ayuda acoke mu Romu; ndipo Paulo anabwela kwa beve; ³ Paulo anankhala nabeve cifukwa benzo cita malando yasemu. Benzo panga matenti. ⁴ So Paulo anakambilana mu sinagoge Sabata iliyonse. Anasimikizila Ayuda naba Giliki. ⁵ Koma pamene Sailasi na Timoti anabwela kucoka ku Mesedoniya, Paulo anauziwa na Mzimu kuti apeleke umboni kui Ayuda kuti Yesu ndiye Kristu. ⁶ Pamene Ayuda banamususha nomunyoza, Paulo anakunkhumula malaya yake kuli beve nokamba ati, "Lekani mwazi wanu unkhale pamitu wanu; Ine nilibe mulandu. Kucokela lero nizayenda kwa akunja." ⁷ Pamene apo anacoka noyenda kunyumba ya Titiyasi Jasitasi, mwamuna enzo lambila Mulungu. Nyumba yake yenze pafupi na Sinagoge. ⁸ Khirisipasi, msogoleli wa sinagoge nanyumba yake yonse anakhulupila mwa Ambuye. Bambila baku Korinto bamene anamvela Paulo anakhulupilila nobatizika. ⁹ Ambuye anakamba ati kwa Paulo usiku mumaso mphenya, Usayope, kamba ndipo usankhale cete. ¹⁰ Cifukwa nilinaiwe, ndipo kulibe azayesa kukucita ngozi, cifukwa ninabanthu bambili mu tauni iyi." ¹¹ Paulo anankhalamo caka cimozi na myezi ili 6, kuphunzisa mau ya Mulungu pakati pawo. ¹² Koma pamene Galiyo anankhala govana wakuAkaya, Ayuda bonse pamozi anaukila Paulo nomuleta pamupando waciweluzo, ¹³ nokamba ati, "Uyu mwamuna akoka banthu luti alambile Mulungu mosushana nalamulo." ¹⁴ Ndipo pamene Paulo enzo funa kukamba, Galiyo anakamba ati kuli ba Yuda, "Imwe Ayuda, ngati yenzeli nkhanu ya cinthu coipa or mulandu, sembe cezebwinu kuku diling'ani. ¹⁵ Koma cifukwa cakuti aya nima funso pa mau nama zina nalamulo yanu, kambalanani. Sinifuna kunkhala oweluzo pali izi nkhanu." ¹⁶ Galiyo anabacosa pamupando oweluzila. ¹⁷ so bonse banagwila Sosithenesi, olamulila sinagoge, nomumenya pasogolo pamupando oweluzila. Koma Galiyo sanafakileko nzeru pavamene anacita. ¹⁸ Paulo ponkhalako masiku yambili, anabasiya abale noyenda ku Siliya pamozi na Prisila na Akwila. Akalibe ucoka pokwelela boti, Kensiriya anagelewa mumutu wake cifukwa enze anapanga pagano yamu Nazareti. ¹⁹ Pamene anafika kwa Aifenso, Paulo anasiya Prisila na Akwila kuja, koma iye anayenda mu sinagoge nokambilana na Ayuda. ²⁰ Pamene banapempha Paulo kuti ankhaleko nthawi itali, anakana. ²¹ Koma pocokapo pali beve, anakamba ati, "Nizabwela futi kwa imwe ngati nicifuniro ca Mulungu." Anabwela acoka kwa Aifenso. ²² Pamene Paulo anafika ku Sizariya, anayenda kupasa moni mupingo waku Yelusalemu nobwelo yenda ku Antioku. ²³ Pamene anakhalako pakanthawi, Paulo anacoka nopitila kumizinda ya Galatiya na Friyiya nolibika ophunzila bonse. ²⁴ Manje mu Yuda winangu zina lake Apolosi wobadwila ku Alekizanda, anabwela ku Aifenso. Enzo ziba bwino mumakambidwe ndiponso namalemba enzo yaziba bwino. ²⁵ Apolosi anaphunzisiwa muziphunziso za Ambuye. Pakunkhala wa cangu mwa yeve, anaphunzisa bwino zinthu zokhuzana na Yesu, koma enzo ziba cabe ubatizo wa Yohane. ²⁶ Apolosi anayamba kukamba molimbika mu sinagoge. Koma pamene Prisila na Akwila anamumvera, anamupanga muzawo nomufotokozela njila ya Mulungu bwini bwino. ²⁷ Pamene anafuna kupitila ku Akaya, ba bale anamulimbikisa nolembela ophunzila baku Akaya kuti amulandile. Pamene anafika, anathandizila maningi baja bamene anakhulupilila mwa cisomo. ²⁸ Apolosi anagonjesa Ayuda benangu pamenso pabanthu namakambidwe yosusha bwino na ukwaswili wake mumakambidwe; mukuwonesela mwa malemba kuti Yesu enzeli Kristu.

Chapter 19

¹ Cinabwela cacitika kuti pamene Apolosi enzeli ku Korinto, Paulo anapitila kuziko yakumwamba nofika ku tauni ya Aifenso, nopeza ophunzira benangu. ² Paulo anakamba ati kwa beve, Bushe munalandila Mzimu Oyela pamene munakhulupilila?" Banakamba ati kwa yeve, "Yayi, sitinamveleko za Mzimu Oyela." ³ Paulo anakamba ati, "Bushe munabatizika mucani?" Banakamba ati "Mu ubatizo wa Yohane." ⁴ So Paulo anayankha ati, Yohane anabatiza ubatizo wotembenuka. Anauza banthu kuti afunik kukhulupila muli yeve wamene azabwela yeve akacoka, umu ndiye mwa Yesu." ⁵ Pamene banthu banamvela izi, banabatizika muzina la Ambuye Yesu. ⁶ Ndipo pamene Paulo anaika manja yake pali beve, Mzimu Oyela anabwela pali Beve ndipo anakamba mubvitundu vinangu nobwela ucita uneneri. ⁷ Namba yonse pamozi enzeli azibabo bali 12. ⁸ Paulo anangena mu Sinagoge nokamba molimbika kwa myezi itatu. Ozosogolela zokambilana nakusimikizila banthu pazinthu zokhuzana na ufumu wa Mulungu. ⁹ Koma pamene Ayuda benangu banalimbisa mtima nakukhala osamvelera, banayamba kukamba voipa pa njila ya Kristu pamenso ya gulu. So Paulo anacokapo pali beve nocosapo wokhulupilila. Anayamba kukamba siku na siku mukilasi ya Tiranasi. ¹⁰ Ici cinapitiliza kwa zaka zibili, mpaka bonse wonkhala mu Asia anamvela mau ya Ambuye, Ayuda na Agiliki pamozi. ¹¹ Mulungu enzocita vinthu vikulu kupitila kumanja ya Paulo, ¹² kuti ngankhale wodwala benzopola, mizimu yoipa yenzocoka muli beve, pamene benzotenga tunyula pa thupi ya Paulo. ¹³ Koma kwenzeli wocosa vibanda baci Yuda benzoyenda kupitila kuja kumalo bamene anatenga zina la Yesu kuyisebenzesa mwacabe. Banayikamba pali baja benzeli na mizimu yoipa; banakamba ati, "Nikulamulila muzina la Yesu wamene Paulo alalikila kuti ucoke." ¹⁴ Aba banacita ici benzeli bana ba wansembe mukulu, Sikeva. ¹⁵ Muzimu onyasa unabayankha, Yesu nimuziba, na Paulo nimuziba; Koma nanga ndiwe ndani iwe?" ¹⁶ Muzimu oyipa unali mu munthu uja unabajumpila baja ocosa vibanda nowapambana mphanvu nobamenya. Banathaba kucoka munyumba muja cinthaku nabvilonda. ¹⁷ Ici canizibika kuli bonse, baci Yuda naci Giliki bonse, benzonkhala mu Aifenso. Banankhala na mantha maningi, ndipo zina ya Ambuye Yesu enalemekezeka. ¹⁸ Ndiponso, bambili okhulupila banalapa nobvumela voipa vamenze enze anacita. ¹⁹ Bambili benzocita vamagiki banaleta mabuku yawo noyashoka pamenso ya aliyense. Pamene banabelengela mtengo wake yenze inakwana fifite sauzande mapisi ya siliva. ²⁰ So mau ya ambuye yanayenda maningi munjila yamphanvu. ²¹ Manje pamene Paulo anasiliza utumiki wake mu Aifenso, anacipanga mumzimu kuti apitile ku Mesedoniya na Akaya pamene enzo yenda ku Yelusalemu; anakamba ati, "Nikankhalako nkhalako, nifunika kuyenda ku Romu." ²² Paulo anatuma ku Mesedoniya ophunzila bake babili, Timoteyo na Erasitasi, bamene benze banamuthandiza. Koma yeve anasala ku Asia pakanthawi. ²³ Panthawi yamene ija kunauka msokonezo mu Aifenso kukhuzana na cikristu. ²⁴ Winangug wopanga vumba kucokela ku siliva zina lake Demetiriyasi, amene anapanga coumba ca Diana, zinamupangila maningi malonda uyu opanga vumba. ²⁵ So anabwelesa pamozi banyanchito bonse pancito ija nchito nokamba ati, "Azikulu, muziba kuti iyi buzinesi imatipangla ndalama. ²⁶ Muona nomvela izi, osati cabe ku Aifenso, koma pafupi fupi mu Asia monse, uyu Paulo wadonsa notembenuka banthu bambili. Akamba kuti kulibe milungu yopangiwa namanja. ²⁷ Sikuzankhala cabe kuti malonda yathu siyazafuniwa, komanso kuti tempele ya mukulu mulungu mukazi Diana ezayesewa ilibe nchito. Nakuti azalusing'a ukulu wake, wamene Asia yonse naziko yonse apembeza." ²⁸ Pamene bamvela izi, banakalipa nolila, "Mukulu ni Diana waku Aifenso." ²⁹ Tauni yonse mwenze musokonezo, ndipo bathu banathabila pamozi mu holo. Banagwila benzo yenda na Paulo, Gayasi, na Aristakasi, bamene banacoka ku Mesedoniya. ³⁰ Paulo anafuna kungena pamozi nacigulu, koma ophunzila banabalesa. ³¹ Cimozi mozi bakulu bakulu bamuzinda wamu Asia bamene benzeli bazake banamutumila uthenga kumupempha kuti asalobe mu holo. ³² Banthu binangu benzo punda cinthu cimozi, cifukwa gulu yenze mumusokonezo. Bambili ba iwo sanazibe cifukwa nicani banabwela pamozi. ³³ Ba Yuda banacosesa Alekizanda pacigulupu kumuyika pasogolo pabanthu. Alekizanda ananyamula kwanja kwake kuti abafotokozele banthu. ³⁴ Koma pamene banaziba kuti ni Yuda, bonse banalila na mau yamozi kwa 2 awazi, "Mukulu ni Diana wabanthu baku Aifenso." ³⁵ Pamene kalaliki watauni anauza banthu kuti ankhale zii, anakamba ati, Imwe bamuna baku Aifenso, nindani munthu wamene saziba kuti tauni ya Aifenso ni tempele yamene isunga mukulu Diana navonsema vamenze vinagwa kumwamba? ³⁶ Kuwona kuti izi zinthu sizingakaniwe, nkhalani zii, ndipo musathamangile. ³⁷ Cifukwa mwaleta aba banthu kukhoti bamene sibakawalala wamu tempele kapena onyozela mulungu wathu mukazi. ³⁸ Cifukwa ca ici, ngati Demetiriyasi nabaja osemi bamene ali nayeve bali nayeve mulandu, makhoti niyoseguka ndipo oweluza baliko. Lekani bapasane milandu beka beka. ³⁹ Koma ngati usakila nkhani zinangu, zizakambiwa mumisonkhano yanthawi na nthawi. ⁴⁰ Cifukwa zoonadi tili padenja kupasiwa mulandu pacongo cacitika lero. Palibe coyofya pali ici congo, ndipo sitizakwanisa kuvifotokoza." ⁴¹ Pamene anakamba izi, anang'ondola musonkhano.

Chapter 20

¹ Pamene rayoti inasila, Paulo anaitana ophunzila ndipo anabalimbiksa. Ndipo anabalayila noyenda ku Mesedoniya. ² Pamene anapitila mizinda ayo nolimbikisa okhulupila maningi, anangena mu Girisi. ³ Pamene anankhalako myezi itatu kuja, kumu ukila kunapangiwa na Ayuda nishi wankhala pang'ono kuyenda ku Siliya, so anaganiza kubwelela kupitila ku Mesedoniya. ⁴ Kumupelekeza iye kufika ku Asia enzeli Sopata mwana mwamuna wa Filasi ocokela ku Beriya; Arisitakasi na Sekundasi, bonse ocokela kwa okhulupila waku Thesalonika; Gayesi waku Debi, Timoti' na Ticikasi na Trofimasi ocokela ku Asia. ⁵ Koma aba banthu banasogolako ndipo benzo tiyembekeza ku Tiraosi. ⁶ Tinayenda kucoka ku Filipi pambuyo pacikodwelelo ca pasaka, ndipo pamasiku yali 5 tinabwelela kwa iwo ku Tiraosi. Kuja tinankhalako masiku 7. ⁷ Siku yoyamba mu sabata, pamene tinakumana pamozi kti tinyemela buredi, Paulo anakamba kuli wokhulupilila. Enzo pulana kuyenda siku yokokhapo, so anapitiliza kukamba mpaka pakati pa usiku. ⁸ Kunali manyale yambili mucipinda capa mwamba mwamene tinakumana. ⁹ Pa windo panankhala Munyamata wingu zina yake Utikasi. wamene anagona maningi. Pamene Paulo anatenga nthawi itali kukamba, uyu munyamata, akali gone, anagwa kucoka pamwamba ndipo anamudoba wakufa. ¹⁰ Koma pamene Paulo anayenda pansi, Paulo anamugonela yeve, numukumbatila. Ndipo anakamba ati, osakalipa futi, cifukwa ali moyo." ¹¹ So anayenda pamwamba futi nonyema buredi nakudya. Pamene anakamba nabeve nthawi itali nishi kufuna kucha, anayenda. ¹² Anamubwelesa munyamata wa moyo ndipo anatohozidwa maningi. ¹³ Ise bamene tinayenda pasogolo pali Paulo na boti noyenda ku Asosi, kwamene tinaganiza kuti tiyenda nayeve Paulo. Ici ndiye camene anafuna yeve kucita, cifukwa anapulana kuyenda pansi. ¹⁴ Pamene tinakumana nayeve ku Asosi, tinamutenga mu boti ndipo tinayenda ku Mitileni. ¹⁵ Tinayenda kucoka paja nofika siku yokokhapo pafupi na pamalo ya Chiyosi. Siku yokokhapo tinafika pamalo ya Samosi, ndipo siku yokokhapo tinafika ku tauni ya Miletasi. ¹⁶ Cifukwa Paulo anagaza kuyenda kupitilila Aifenso, kuti asataye nthawi ili yonse mu Asia; cifukwa enzo thamangila ku Yelusalemu kuti apezekoko ku siku ya Pentekositi, kati cenzeli cokwanilisika kwa yeve kucita so. ¹⁷ Kucoka ku Miletasi anatuma banthu ku Aifenso ndipo anaitana akulu amu mpingo. ¹⁸ Pamene anabwela kuli yeve, anakamba ati kuli beve, kucoka siku yoyamba pamene ninangena mu Asia, mwamne lyonse nimakhallila na imwe. ¹⁹ Ninapitiliza kutumikila Ambuye mozicepesa na misozi, namasauso yamene yananicitikila ine cifukwa ca kuniteya kwa Yuda. ²⁰ Muziba mwamene sinina nkhalile zii pakukuuzani camene cinali cofunikila, namwamene ninakuphunzilisani pagulupu nakupitamo muma nyumba. ²¹ Muziba mwamene ninapitiliza kucenjeza ba Yuda naba Giliki pakutembenukila kuli Mulungu na cikhulupililo mwa Ambuye Yesu. ²² Koma manje, onani, niyenda omangiwa mu Mzimu Oyela ku Yeslusalemu, siniziba zamene zizanicitikila kuja, ²³ kucosako cabe kuti Mzimu Oyela amakamba naine mu tauni iliyonse nokamba ati macheni nakubvutika kuku yembekezela. ²⁴ Koma sinibelengela kuti umoyo wanga niwabwino kwa ine, kuti nisilize nchito yanga nautumiki wamene ninalandila kucokela kwa Ambuye Yesu, kuti nipeleke umboni pali uthenga wa cisomo ca Mulungu. ²⁵ Ndipo manje, onani, niziba kuti monse, bamene ninapitamo kulalikila za ufumu, simuzaniwona futi. ²⁶ Cifukwa ca ici nipelekela umboni kwa imwe lero, kuti nilibe mulandu pa mwazi wamunthu aliyense. ²⁷ Cifukwa sininankhale zii kukamba kwa imwe cifunilo conse ca Mulungu. ²⁸ So nkhalani ozisamalila imwe mweka, na nkhusa zonse zamene Mzimu Oyela anakupanga kunkhala oyanganila. Nkhalani osamalila kucita ubusa pa mpingo wa Mulungu wamene anagula na mwazi wake. (Malemba yenangu yakamba ati, Nkhalani ocenjela kusamalila mupingo wa Mulungu wamene anagula namwazi wa mwana wake). ²⁹ Niziba kuti ngati nacoka, mimbulu yolusa izaloba pakati panu, ndipo si izalekelela nkhusa. ³⁰ Niziba kuti ngankhale pakati panu bamuna binangu azabwela nokamba vinthu voononga, kuti bakoke ophunzila kuli beve. ³¹ So nkhalani pa gadi. Kumbukilani kuti kwa zaka zitatu sininaleke kuuza aliyense wa imwe vocita namisozi usiku na muzuba. ³² Manje nikupelekani kwa Mulungu nakumau yacisomo cake, yamene yakwanisa kukumangani imwe ndiponso kukupasani colowa pakati pabonse bamene bali oyelesedwa. ³³ Sininakhubwile siliva, golide kapena malaya yamunthu. ³⁴ Imwe mweka muziba kuti mwanja yanga yanapipasa zamene nezofuna nazofuna zabaja bamene nenzeli nabo. ³⁵ Muzinthu zonse ninakupasani cisanzo mwamene mufunikila kuthandizila ofoka pakusebenza, namwamene mufunikila kukumbukila mau ya Ambuye yesu, mau yamene yeve yeka anakamba: "nikodalisika kupasa kupambana kulandila." ³⁶ Pamene anakamba munjila yaso, anagwada pansi nopemphela nabo pamozi bonse. ³⁷ Bonse banalila maningi nomukumbata mumkosi nomu kising'a. ³⁸ Banamvela cifundo maka maka pazamene anakamba, kuti sazamuwonanso. Ndipo anamupelekeza ku boti.

Chapter 21

¹ Pamene anacoka pali beve nobwelo yambapo, tinayenda njila ya siteleti ku tauni ya Kosi, ndipo siku yokokhapo ku tauni ya Rodesi, ndipo kucoka apo ku tauni ya Patara. ² Pamene tinapeza boti itauka kuyenda ku Fonisiya, tinakwelamo nobwelo yambapo. ³ Pamene tinabona mzinda wa Sipurasi, tinausiya ku mazele, noyenda ku Siliya, ndipo tinafika pa tauni ya Taya, cifukwa ndiye kwamene boti yenzofunika kusiya katundu. ⁴ Pamene tinapeza ophunzila, tinakhalako masiku yali 7. Aba bophunzila banakamba ati kuli Paulo kupitila mwa Mzimu kuti safunika kudyekamo kwendo mu Yelusalemu. ⁵ Pamene masiku yanasila, tinacoka nopitiliza na ulendo wathu. Bonse, pamozi nabazikazi nabana bawo, anatipelekeza mpaka ninacoka mu tauni. Ndipo tinagwada mumbala yamumana, nopemphelela, nolailana wina namuzake. ⁶ Tinakwela boti, pamene beve benzo bwelelanso kunyumba. ⁷ Pamene tinasiliza ulendo waku Taya, tinafika pa Ptolemasi. Luja ninapasa moni abale nonkhalako siku imozi. ⁸ Siku yokokhapo tinacoka noyenda ku Sezariya. Tinangena mu nyumba ya Filipo, mlaliki wa uthenga, wamene anali umozi pali baja 7, ndipo tinankhala naye. ⁹ Manje uyu mwamuna enzeli naba namwali bali 4 bamene benzo nenera. ¹⁰ Pamene banakhalako kuja kwa siku, Kunabwela kucoka ku Judeya mneneri winangu zina lake ni Agabasi. ¹¹ Anabwela kwa ise notenga beoti ya Paulo. Anazimanga nayo mendo na manja yake nokamba ati, "Icindiye camene akamba Mzimu Oyela, 'Cimuzi mozi ndiye mwamene azacitila Ayuda mu Yelusalemu kumanga mwinewake wa beoti iyi, ndipo azamupeleka mumanja ya Akunja.'" ¹² Pamene tinamvela izi zinthu, ise pamozi nabaja banthu benzonkhala malo yaja tinamupepha Paulo kuti asayendeko ku Yelusalemu. ¹³ Koma Paulo anayankha, "Mucita cani, kulila nobabisa mtima wanga? Cifukwa ndine okonzekela, osati kumangidwa cabe koma kumwalila mu Yelusalemu cifukwa ca zina la Ambuye Yesu." ¹⁴ Cifukwa Paulo sanafune kugonjela, tinaleka kumulesa ndipo tinakamba ati, Lekani cifunilo ca Ambuye cicitike." ¹⁵ Pamene masiku aya yanasila, tinatenga viola vathu noyenda ku Yelusalemu. ¹⁶ Kuja nakwebve anayendela naise pamozi ophunzira ocokela ku Sezeriya. Anabwela namunthu zina lake ni Mnasoni, mwamuna ocokela ku Sipurasi, ophunzila oyamba, wamene tenzonkhala nayeve. ¹⁷ Pamene tinafika mu Yelusalemu, ba bale banatiladila mokodwela. ¹⁸ Siku yokokhapo Paulo anayenda naise kuli Jemusi, ndipo akulu bonse benzelipo. ¹⁹ Pamene anabapasa moni anarepota umozi, umozi vinthu vamene Mulungu anacita pakati pali Akunja kupitila mu utumiki wake. ²⁰ Pamene banazimvela, banayaminka Mulungu, ndipo banakamba ati kwa yeve, "Woonna, mubale, nibangati ma sauzande bamene bakhulupilila pakati pali Ayuda. Bonse nibofunisisa kusunga malamulo. ²¹ Banauziwa za iwe, kuti uphunzisa a yuda bonse bamene ankhala pakati pa Akunja kuti aleke Mose, ndipo kuti ubabuza kuti asacite mdulidwe bana bawo, ndipo kuti basakonkhe mwambo wakudala. ²² Kansi nizacita bwanji? Bazamvela kuti unabwela. ²³ So cita camene tikuuza manje: nina bamuna bali 4 bamene banapanga pangano. ²⁴ Tenga aba banthu ndipo uziyelese wake pamozi nabeve, ndipo ubalipilile, kuti agele mitu yawo. Kutu wina aliyense azibe kuti vinthu vamene banauziwa pali iwe nivaboza. Bazaziba kuti naiwenso uknkha lamulo. ²⁵ Koma pali ba Kunja bamene banakhulupilila, tinabalembela kubauza kuti bazisunge kuvinthu vopelekewa ku mafano, mwazi, cakufa ceka na ciwele wele." ²⁶ Ndipo Paulo anatenga baja bamuna, ndipo siku yokokhapo, anaziyelesa yeve na beve, analoba mu tempele nonaunsa masiku yakuyesedwa, paka copeleka cinapelekwedwa kwa beve bonse. ²⁷ Pamene masiku yali 7 yanankhala pang'ono kusila, Ayuda baku Asia banona Paulo mu tempele, ndipo anatufya bonse kuti bapange congo, ndipo banamugwila yeve. ²⁸ Benzo punda, "Bamuna ba Israyeli, tithandizeni. Uyu ndiye munthu wamene aphunzisa banthu bonse vinthu vosushana na banthu, lamulo na malo yano. Kucosapo izi, anabwelesanso a Giliki mu tempele nofifya malo aya yoyela." ²⁹ Cifukwa banaonapo Trofimas waku Aifenso nayeve mu tauni, ndipo banganiza kuti kapena Paulo ndiye anamuleta mu tempele. ³⁰ Tauni yonse inakalipa, ndipo banthu banathamanga pamozi nomugwila Paulo. Banamucosa mu tempele, ndipo viseko vinavaliwa pamene apo. ³¹ Pamene benzo yesa kumupaya, nkhanu inafika kuli capitawo mukulu wama gadi kuti Yelusalemu yonse yenze mucongo. ³² Pamene apo anatenga asilikali nothamangila kwamene kwenze gulu. Pamene gulu inawona kapitawo mukulu na asilikali, banaleka kumumenya Paulo. ³³ Pamene apo kapitawo mukulu anafika nogwila Paulo, nolamulila kuti amagidwe na macheni yabili. Banamufunsa kuti iye nindani nacamene wacita. ³⁴ Banthu benangu mucigulu benzo punda ici benagu cija. Cifukwa cakuti kapitawo sanazibe cokamba cifukwa cacongo, analamulila kuti Paulo apelekewe mumalo yothabila. ³⁵ Pamene anafika pama sitepu yamalo pothabila, asilikali banamunyamula cifukwa ca congo ca gulu. ³⁶ Cifukwa gulu inakonkha ndipo benzo punda kuti, "Sitimufuna yeve!" ³⁷ Pamene anankhala pang'ono Paulo kuti afika pa malo yothabila, anakamba ati kuli kapitawo mukulu, "Kansi ningakambeko cinthu cinangu kwa iwe?" Kapitawo anakamba ati, umakamba ci Giliki? ³⁸ Sindiwe waku Egypto, wamene manje manje apa unaleta ku ukila notenga bowukila bali 4 sauzande mucipululu?" ³⁹ Paulo anakamba ati, Ndine mu Yuda, kucoka ku tauni ya Tarsasi mu Silisiya. Ndine sitizeni wa tauni yofunikila. Nikupempha, nilole nikambe nabanthu." ⁴⁰ Pamene kapitawo mukula anamubvomeleza, Paulo

anaimilila pama sitepu nonyamula kwanja kubanthu. Pamene kunankhala zii maningi, anakamba na yeve mucu Heberi. Anakamba ati,

Chapter 22

¹ "Abale na batate, mvelani kuzidifenda kwanga kwamene nipeleka kwa imwe." ² Pamene gulu inamvela Paulo kukamba nabeve mucitundu caci Heberi, banankhala zii. Anakamba ati, ³ Ndine mu Yuda, obadwila mu Tasasi ku Silisiya, koma ophunzilila mu tauni ino kuli Gamaliyelo. Ninaphunzisiwa kulingana na njila zacilamulo zamakolo bathu. Ndine wacangu pali Mulungu, monga mwamene mulili imwe monse lero. ⁴ Ninasausa ba kristu kufika nopaya; ninamanga bamuna nabakazi pamozi nobapeleka mujele. ⁵ Ndipo mkulu wa nsembe na azikulu angapelekele umboni kuti ninalandila makalata kucoka kuli beve pali ba bale ali ku Damasikasi, kuti ine niyende kuja. Nenzo funika kuleta akristu womangidwa ku Yelusalemu kuti bapanishiwe. ⁶ Cinacitika kuti pamene nenzo yenda nonkhala pafupi na Damasiko, camuzuba mwazizi laiti ikulu kucoka kumwamba inasanika kuzunguluka ine. ⁷ Ninagwa pansi nakumvela mau kukamba naine, 'Sauli, Sauli, nicifukwa nicicani unasausa ine?' ⁸ Ninayankha, Ndimwe ndani Ambuye?' Anakamba naine kuti, 'Ndine Yesu waku Nazareti, wamene unzuna.' ⁹ Baja bamene anali naine banaiwona laiti, koma sibanamvesese mau yauja wamene anakamba naine. ¹⁰ Ninakamba ati, Nicite bwabji, Ambuye?' Ambuye anakamba naine ati, 'Nyamuke uyende ku Damasikasi; kuja uzauziwa zonse zamene ufunika kucita.' ¹¹ Sinenzo kwanisa kubona cifukwa ca kuyaka ca laiti ija, so ninayenda ku Damasikasi kusogolelewa nabaja wamene enzeli na ine. ¹² Kuja ninakuma namwamuna zina lake ni Ananiyasi, mwamuna ozipoleka kulingana nalamulo ndipo ba Yuda bonse bonkhala kuja banakamba zabwino pali yeve. ¹³ Anabwela kwa ine, noimila pafupi naine, nokamba ati, 'Mubale Sauli, landila maso yako.' Munthawi yamene iwo ninayangana. ¹⁴ Ndipo anakamba ati, Mulungu wamakolo yathu akusankha iwe kuti uzibe cifunilo cake, kuti uwone Iye Olungama, ndipo kuti umvele mau yocokela pakamwa pake. ¹⁵ Cifukwa uzankhala mboni yake kubanthu bonse pazamene waona nomvela. ¹⁶ Manje nicifukwa nicanu uyembekezela? Nyamuka, nobatizika, nosunka macimo yako, kuitana pazina lake.' ¹⁷ Pamene ninabwelela ku Yelusalemu, ndipo pamene nenzopemphela mu tempele, cinacitika kuti ninapasiwa maso mphenya. ¹⁸ Ninamuwona akamba naine, Indisa yenda ku Yelusalemu mwamusanga, cifukwa sibazalandila umboni wako pali ine.' ¹⁹ Ninakamba ati, Ambuye beve beka baziba kuti ninamanga nomenya baja bamene anakhulupilila mwa imwe mu sinagoge ili yonse. ²⁰ Pamene mwazi wa Stefano mboni yanu unatika, nenzo yembekezela nogwilizana nazo, ndipo nizogading'a malaya baja bamene anamupaya.' ²¹ Koma anakamba ati kwa ine, 'Yenda, cifukwa nizakutuma kwa Akunja.' ²² Banthu banamulo kuti akambe kufika apa. Koma banapunda nokamba ati, Mupayeni sitimufuna pano pacalo: sicofunikila kuti ankhale na moyo." ²³ Pamene benzeli kupunda, kumuponyela malaya yabo, noponya kalukungu mumwamba, ²⁴ kapitawo mukulu analamulila kuti Paulo apelekewe mu malo yothabila. Analamulila kuti afunsiwe namikwapu pamene, kuti yeve aziba nicifukwa nicanu benzo pundila yeve monga so. ²⁵ Pamene banamumanga navinthambo, Paulo anakamba kuli musilikali wamene enze cilili pafupi, Kansi nicololedwa kukwapula munthu wamene ni mu Roma ndipo wamene sanaweluzidwe?" ²⁶ Pamene musilikali anamvela izi, anayenda kuli kapitawo mukulu nomuza kuti, kansi ufuna ucite canu? Uyu munthu ni sitizeni waku Roma. ²⁷ Kapitawo mukulu anabwela nokamba ati kwa yeve, "Niuze, ndiwe sitizeni waku Roma?" Paulo anayankha ati, "Inde." ²⁸ Kapitawo mukulu anayankha ati, "ninasebenzesa ndalama zambili kuti ninkhale sitizeni." Koma Paulo anakamba ati, ine ninabadwa sitizeni wa Roma." ²⁹ Ndipo banthu benzo yenda umufunsa banamusiya pamene apo. Kapitawo mukulu nayeve anayopa, pamene anaziba kuti Paulo enze sitizeni wa Roma, cifukwa anazimangilila yeka. ³⁰ Siku yokokhapo, kapitawo mukulu enzofuna kuziba coonadi pali mulandu wamene Ayuda anapasa Paulo. So anamumasula nalamulila akulu asembe na khanso yonse kuti bakumane. Pamene apo analeta Paulo nomuyika pakati pawo.

Chapter 23

¹ Paulo anayangana pali ma membala ba nkhanso nokamba ati, "Abale, nankhala pamaso pa Mulungu mumaganizo abwino kufikila lelo." ² Mukulu wa nsembe Ananiyasi analamulila baja bamene naimilila pafupi nayeve kuti amumenye pakamwa. ³ Ndipo Paulo anakamba ati kwa yeve, Mulungu azakumenya iwe, iwe cipilala ca waiti. Kansi wankhala kuniweluzwa ine mwa lamulo, koma ulamulila kuti banimenye, mosushana na lamulo?" ⁴ Baja bamene banaimilila pafupi banakamba ati, "Umu ndiye mwamene unyozela mukulu wansembe wa Mulungu?" ⁵ Paulo anati, Sininanyozele, abale, kuti enzeli mukulu wa nsembe. Cifukwa kunalembewa, Suzakamba zoipa pali wolamulila wa banthu bako." ⁶ Pamene Paulo anabona kuti mbali imozi yaba khanso anali a saduki ndipo mbali imozi apharise, anakamba mopunda mu khanso, "Abale, ndine Mupharise, mwana mwamuna wa Mupharise. Nicifukwa cakuti nilinaco cisimikizo kuyembekezela bakufa kuuka ndiye camene niweluziliwa." ⁷ Pamene anakamba izi, kusushana pakati pa Apharise na Saduki kunayamba, ndipo gulu inagabikana. ⁸ Cifukwa Asaduki akamba kuti kulibe kuuka, kulibe angelo, namizimu, koma Apharise bagwilizana nazo zonse. ⁹ So mukangano ukulu unacitika, ndipo olemba binangu benzeli kumbali ya Pharisi anaimilila nosusha, kukamba kuti, "Sitipeza mulandu nauyu munthu. Nanga ngati muzimu kapena mungelo akamba naiye?" ¹⁰ Ndipo apo kunauka kukangana maningi, kapitawo mukulu anayopa kuti Paulo azamupweteka, so analamulila asilikali kuti bamutenge mwacikakamizo pakati pama membara ba khanso, nakumubwelesa pamalo yothabila. ¹¹ Usiku okokhapo Ambuye anaimilila pafupi nayeve nomuuzwa kuti, "Osayopa, monga mwamene wapelekela umboni pali ine mu Yelusalemu, so ufunika kupeleka umboni mu Roma." ¹² Pamene kunakhala kuseni, bena ba Yuda banagwilizana noitana tembelelo pali beve: banakamba ati sibazadya kapena kumwa ciliconse paka maupaye Paulo. ¹³ Benzeli wokwanila ngati bamuna bali 40 bamene banapanga iyi pangano. ¹⁴ Banayenda kuli mukulu wa nsembe na azikulu nokamba ati, tazifaka pa tembelelo ikulu, sitizadya kanthu paka tipaye Paulo. ¹⁵ Manje so, lekani khanso iwuze kapitawo mukulu alete Paulo kuli iwe, cifukwa ungaweluze mulandu wake bwino. Kuli ise, ndise wokonzekela kumupaya iye akalibe kufika kuno." ¹⁶ Koma mwana wa sisita wa Paulo anamvela kuti benzo muyembekezela, so anayenda noloba mumalo yothabilapo numuuzwa Paulo. ¹⁷ Paulo anaitana umozi wa asilikali nokamba ati, "Mupeleke uyu nyamata kuli mukulu wa asilikali, cifukwa ali navamene afuna kumuuzwa." ¹⁸ So musilikali anatenga munyamata nomuleta kuli kapitawo mukulu nokamba ati, Paulo kaidi ananiitanila yeve, noniuzwa kuti nilete uyu munyamata kwa iwe. Alinacokamba kwa iwe." ¹⁹ Kapitawo mukulu anamutenga pakwanja pamalo yobisika nomufunsa, "Ufuna kuniuzwa cani?" ²⁰ Mnyamata anakamba ati, Ayuda bagwilizana kuti bakupemphe kuti ulete Paulo mailo ku khanso, monga ngati bafuna kumufunsa bwino bwino pali uyu mulandu. ²¹ Koma usabvomele, cifukwa kuli bamuna wopitilila bali 40 bamene bamuyembekezela. Bazifaka tembelelo, kuti sibazadya kapena kumwa mpaka bamupaye Paulo. Namanje so, niwokonzekela, kuyembekezela kuti ubvomele." ²² So kapitawo mukulu anamusiya mnyamata kuti ayende, nishi amuuzwa kuti, "Usauze aliyense kuti waniuzwa izi zinthu." ²³ Pamene apo anamuitanila asilikali babili nokamba ati, Konzekelani basilikali bali 200 kuti bayende ku Sezariya, nabali 70 bamahosi, nabamikondo bali 200. Muzayenda na 9:00 koloko." ²⁴ Anabalamulila kuti bamupase nyama yamene Paulo aza yenzanomupeleka kuli govana Felike. ²⁵ Ndipo analembe kalata kuti: ²⁶ Klaudiyasi Lisiyasi kuli olemekezeka Govana Felike, nikupasa moni. ²⁷ Uyu munthu anamagidwa na Ayuda ndipo enzofuna upaiwa nabeve, pamene apo tinabwela nabasilikali nomumasula, cifukwa ninamvela kuti enzeli sitizeni waku Roma. ²⁸ Ninafuna kuziba camene banamupasila mulando, so ninamupeleka ku khanso yabo. ²⁹ Ninabwela kuti banamupasa mulandu pamafunso ya malamulo tabo, koma kwenzelibe mulandu pali yeve wenzofunika kui bamupaye kapena kumufaka mujele. ³⁰ So ninazibisiwa kuti penzeli pangano pali uyu munthu, so mwamusanga musanga ninamutuma kuli imwe, ndipo ninauza womupasa mulandu kuti balete milandu zake kuli imwe. Bayi." ³¹ So asilikali anabvelela kulamulila kwawo: banatena Paulo usiku nomuleta kuli Antipatirisi. ³² Siku yokokhapo, basilikali bambili anasiya baja benzeli pamahosi kuti bayende nayeve ndipo beve babwelele kumalo yothabilapo. ³³ Pamene baja benzeli pamahosi banafika Sezariya nopeleka kalata kuli govana, ndiponso banapeleka Paulo kuli yeve. ³⁴ Pamene govana anabelenga kalata, anafunsa kumuzinda kwamene Paulo anacokela; pamene anamvela kuti anacokela ku Silisiya, ³⁵ anakamba ati, nizakubwela mofikapo pamene bamene bakupasa mulandu bafika." So analamulila kuti bamusungile mu hedikota yaboma ya Herode.

Chapter 24

¹ Patapita masiku 5, Ananiyasi mukulu wansembe, akule bena, na loya zina lake Tetulasi, anayendako kuja. Aba banthu banaleta milndu ya Paulo kuli govana. ² Pamene Paulo anaimilila pamenso pa govna, Tetulasi anayamba kumupasa mulandu nokamba ati kuli govana, "Cifukwa ca iwe tinamutendele ukulu, ndipo masomphenya yako yatiletela kusinthika muziko yathu; ³ so nacyamiko consetilandila zonse zamene ucita, wolemekezeka Felike. ⁴ Kuti nisakusungeni futi, nipempha kuti mwamusanga munimvele mokoma mtima. ⁵ Cifukwa napeza uyu munthu kunkhala kantha ta nawamene apanga Ayuda bonse paziko yonse kuti baukile. Nimusogoleli wa kagulu kaba Nazarene. ⁶ Enzo funa nonyoza tempele, so tinamumanga. (Ndipo tenzofuna kumumanga kulingana na lamulo). ⁷ (Koma Lisiyasi ofisala, anabwela ndipo mwacikakamizo anamutenga mumanja mwathu). ⁸ Pamene munamunsa Paulo pali zonse nkhanu, imwe, naimwe, muzaziba vamene timupasila milandu." ⁹ Ba Yuda pamozi banamupasa mlandu Paulo, nabeve, nokamba ati izi zinthu nizazoonu. ¹⁰ Koma pamene govana anauza Paulo kuti akambe, Paulo anayankha, Ninamvela kuti paka nthawi katali wankhala oweluzu kucalo icic, ndipo mokondwela nifotokoza izi zinthu kwa iwe. ¹¹ Ukwana kupeza kuti sipana pite masiku 12 pamene ninayenda kulambila ku Yelusalemu; ¹² ndipo pamene ananipeza mu tempele, sininasushane na munthu aliyense, ndipo sininabushe viongo, mumasinagoge olo mu tauni, ¹³ ndipo sibangaku simikizile pa milandu zamene anipasa apa manje. ¹⁴ Koma nibvomela ici kuli iwe, kuti kulingana namwamene baitanila ka gulu kan'ono, munjila yamene iwo nitumikila Mulungu ya azitate bathu. Ndine okhulupililika kulingana nazamene zili mucilamulo novolembewa muli aneneri. ¹⁵ Nili naco cisimikizo ca semu muli Mulungu, monga aba banthu nabeve bacyembekeza, kuukisidwa kwa akufa kwamene kubwela, kwa oulangama nabaja bosalungama; ¹⁶ ndipo mwa ici nisebenza kuti ninkhale namaganizo yalibe vuto pamaso ya Mulungu na banthu muzinthu zonse. ¹⁷ Ndipo pamene panapita zaka zambili ninabwela kuleta thandizo kucalo canga na mphaso za ndalama. ¹⁸ Pamene ninacita ici, Ayuda benangu ocokela ku Asia banipeza mumwambo wozitubisa mu tempele, kwenzelibe gulu kapena ku usha viongo. ¹⁹ Aba banthu bafunika kunkhala pa menso pako manje kuti bakambe zamene bali nazo pali ine, ngati bali nazo. ²⁰ Olo kapena, aba banthu bamene akambe voipa vamene bapeza muli ine pamene ninaimilila pamenso ya khanso Yacyiuda; ²¹ pokhapo ngati cili pali camene nakamba mopunda pamene nenze naimila pali beve, 'nipali kuuka kwa akufa pamene niweluziwa lero naiwe.'" ²² Felike enzeli ozibisiwa bwino pa nkhanu yacikristu, so mulandu anabupeleka pa sogolo. Anakamba ati, "Nthawi iliyonse pamene Lisiyasi olamulila azabwela kucoka ku Yelusalemu, nizaweluzu mulandu wako." ²³ So analamulila musilikali kuti agading'e Paulo, koma ankhole namutendele, ndipo pasankhole aliyense azalisa bazake kumuthandiza kapena kuyendela yeve. ²⁴ Patapita masiku, Felike anabwelela ku Durusila mkazi wake, Wacyiuda, ndipo anaitasa Paulo ndipo anmumvelela mwamene anakambila pa cikhulupililo mwa Kristu Yesu. ²⁵ Koma pamene Paulo anakambilana nayeve pali ciyelo, kuzilesa, naciweluzilo camene cibwela, Felike anankhala namantha nokamba ati, "Coka apa pali ine. Koma nikankala nanhtawi inangu zizakuitana." ²⁶ Panthawi yamene iyo, enzoyembekezela kuti Paulo azamupasa ndalama yeve, so enzomuitana kabili kabili nokamba nayeve. ²⁷ Koma pamene zaka zibili zinapita, Ponshasi Fesitasi anakhala govana pamene Felike anacokapo, koma Felike enzo funa kuti Ayuda bamukonde, so anasiya paulo alioganding'iwa.

Chapter 25

¹ Manje Fesitasi anangene mu mzinda, ndipo patapita masiku yatatu, anayenda kucoka ku Sezariya anafika naku Yelusalemu. ² Mkulu wa nsembe na Yuda bozibika bwino analeta mulandu pali Paulo kwa Fesitasi, ndipo banakambisisa maningi kwa Fesitasi. ³ Ndipo banapempha Fesitasi kuti aba citeko bwino pali Paulo, kuti amuitane kuti abwele ku Yelusalemu kuti bamupayile munjila. ⁴ Koma Fesitasi anayankha kuti Paulo anali kaidi waku Sezariya, ndipo kuti yeve manje manje enzobwelela kuja kwamene. ⁵ "Cifukwa caici, baja bamene bakwanisa," anakamba yeve, afunika kuyende pamozi naise. Ngati pali bvuto iliyonse pali uyu munthu, muzamupasa mulandu." ⁶ Pamene anankhalako masiku 8 olo 10, anayenda ku Sezariya. Nipo pasiku yokonkhapo, anakhala pamupando oweluzila ndipo analamulila kuti Paulo abwele kwa yeve. ⁷ Pamene anafika, Ayuda aku Yelusalemu anaimilila pafupi, ndipo analeta milandu yambili yamene sibana puluve. ⁸ Paulo anazidifenda nokamba ati, "Sininacita kanthu koipa pali lamulo ya Ayuda kapena pali tempele kapena pali Seza." ⁹ Koma Fesitasi anafuna kuti Ayuda amukonde, ndipo anayankha Paulo nokamba ati, "Ufuna uyende ku Yelusalemu kuti nikakuweluzila pali izi zinthu?" ¹⁰ Paulo anakamba, "Ni imilila pamaso pamupandu waciweluzo wa Seza kumwene nifunika kuweluziwa. Sininalakwila Muyuda aliyense, monga iwe uzibila bwino." ¹¹ Koma ngati nacita coipa ndipo nacita camene cifunikila imfa, sinikana kumwalila. Koma ngati palibe milandu, kulibe wamene angani peleke kuli beve. Ni itana Siza." ¹² Pamene Fesitasi anakamba naba Nkhanso, anayankha kuti, waita Siza; uzayenda kuli Siza." ¹³ Patapita masiku, Mfumu Agiripa na Benisi anafika ku Sizariya kuti ayendele mwapadela Fesitasi. ¹⁴ Pamene anankalako masiku yambili, Fesitasi anapeleka nkhanu ya Paulo kuli mfumu; anakamba ati, Munthu winangu anamusiya Feleki kuno monga kaidi. ¹⁵ Pamene nenzeli ku Yelusalemu, mkulu wa nsembe na akulu ba Ayuda analeta milandu kwa ine pali uyu munthu, ndipo banafuna ine kuti nimuweluze. ¹⁶ Pali ici ninayakha kuti simwa mwambo wa Aroma kuweluzila munthu monga mwamene bafunila; koma, koma munthu anamulandu ali namupata kuti akumane nabomupasa mulandu kuti azidifende pali milandu yamene anamupasa. ¹⁷ So, pamene anabwela pamozi kuno, sininayembekezele, koma siku yokonkhapo ninankhala pamupando oweluzila ndipo ninalamulila kuti amulete. ¹⁸ Pamene omupasa mulandu anaimilira nomupasa mulandu, ninanganiza kuti panalibe mulandu wene wene pamilandu yamene anamupasa. ¹⁹ Mmallo mwake, enzeli namukangano nayeve pali cipembezo cawo napali Yesu winangu wamene anafa, wamene Paulo akamba ati alimoyo. ²⁰ Ninasokonezeka mwamene ningafufuzile iyi nkhanu, ndipo ninamufunsa ngati tingayende ku Yelusalemu kuti akaweluzidwe kwamene uko pali izi nkhanu. ²¹ Koma pamene Paulo anapempha kuti aganding'iwe kuti amvele nganizo ya empala, ninalamulila kuti amusunge paka nimutume kuli Siza." ²² Agiripa anakamba na Fesitasi, "Nifuna naine nimumvele uyu munthu." "Mailo," Fesitasi anakamba ati, "Uzakamumvela." ²³ So siku yokonkhapo, Agiripa na Benise anabwela na mwambo maningi; banangene mu holo nasilikali nabanthu bozibika mu tauni. Pamene Fesitasi anakamba lamulo, Paulo anamubwelesa kuli yeve. ²⁴ Fesitasi anakamba ati, "Mfumu Agiripa, naimwe onse amuna muli naise muno, mwamuona uyu munthu; onse gulu ya Ayuda anapempha nzeli kuli ine mu Yelusalemu na kuno nakweve, ndipo anapunda kwa ine kuti asankhale futi na moyo." ²⁵ Ninazindikila kuti sanapange mulando ufunika kupaiwa; koma anaitana empala, ndipo ninaganiza kumutuma. ²⁶ Koma nilibe cene cene kuti nilembele kuli empara. Cifukwa caici, namubwelesa kwa iwe, maka-maka kwa iwe, Mfumu Agiripa, kuti ningankhale navo volemba pali uyu mulandu. ²⁷ Cifukwa sicioneka bwino kwa ine kupeleka kaidi ndiponso kukamba milandu yake."

Chapter 26

¹ So Agiripa anakamba kuli Paulo, "Zikambile iwe weka." So Paulo ananyamula kwanja nozidifenda. ² "Niziyesa okondwela ine neka, Mfumu Agiripa, kuti nikambe mulandu wanga pameso yanu siku yalero kusushana nazonse zamene Ayuda anipasa; ³ makamaka, cifukwa muziba bwino malamulo namafunso yonse ya Yuda. So nipempha kuti mumvelere bwino bwino. ⁴ Zoona, a Yuda onse aziba mwamene ninankhalila kucoka ku ufana wanga muzi ziko yanga namu Yelusalemu. ⁵ Ananiziba kucokela poyamba ndipo afunika kubvomela kuti ndine mu Falisi, kagulupu koikako nzelu pali cipembezo cathu. ⁶ Koma manje niimilila pano kuti niweluziwe cifukwa nisakila lonjezo yamene Mulungu anapanga kuli azitate anthu. ⁷ Cifukwa iyi ndiye lonjezo yamene mitundu ili 12 inayembekeza kulandila pamene enzo yamika Mulungu usiku namu zuba. Nipali ciyembekezo ici, Mfumu Agiripa, yamene Ayuda anipasila mulandu. ⁸ Cifukwa nicani kuti winangu waimwe kuti muganize kuti nicodabwisa kuti Mulungu aukisa akufa. ⁹ Panthawi inangu ninaganiza paine neka kuti nifunika kucita vinthu vambili vosushana nazina ya Yesu waku Nazareti. ¹⁰ Ninacita izi mu Yelusalemu. Nnakhomela okhulupilira ambiri mujele kupitila mu mphabvu zamene ninalandila kucokela kuli mkulu wa nsembe, ndipo pamene anapaiwa, ndipo ninaponya voti yanga kusushana nawo. ¹¹ Ninabapasa cilango nthawi zambiri muma sinagoge ndipo nenzoyesa kubakakamiza kuti anyozele. Ananikwiisa maningi ndipo ninabasausa namumatauni yenangu. ¹² Pamene nenzo cita ivi, ninayenda ku Damasikasi namphavu na malamulo yocokela kwa mkulu wa nsembe; ¹³ ndipo nili munjila, pakati pa siku, Mfumu, ninaona laiti kucoka ku mwamba yamene yenzeli yoyaka maningi monga zuba ndipo inasanika pali ine nabanthu enzoyenda naine. ¹⁴ Pamene tonse tinagwa pansi, ninabvela mau kukamba naine yamene inakamba mucitundu caci Heberi, 'Saulo, Saulo, nicifukwa nicani unisausa ine? Nicovuta kuti iwe umenye Mulungu. ¹⁵ Ndipo ninakamba ati, 'Ndimwe ndani, Ambuye?' Ambuye anayakha, Ndine Yesu wamene usausa. ¹⁶ Manje nyamuka ndipo imilila; cifukwa pa colinga ici ninaonekela kwa iwe, kukusankha kunkhala wanchito namboni pali zinthu zamene uziba pali ine na zinthu zamene nizakuonesha pasogolo pake; ¹⁷ ndipo nizakupulumusa kuli anthu na Akunja kwamene nikutuma, ¹⁸ kuti ukasegule menso yabo nobatembenula kucoka ku mdima kubaleta ku laita ndipo kucoka kuli satana kubabwelesa kwa Mulungu, kuti bangalandile Mulungu nakukhululukiwa macimo nakatundu wamene nibapasa wamene nipatula kwa ine mwacikhulupiliro mwa ine. ¹⁹ Cifukwa caici, Mfumu Agiripa, sindinacitile mwano maso mphenya yakumwamba; ²⁰ koma kwa iwo aku Damasikasi coyamba, wokokhapo ku Yelusalemu, ndipo namuziko yonse ya Yudeya, ndiponso na Akunja, ninalalikila kuti atembenuke kwa Mulungu, cocita zinthu zoyenela kulapa. ²¹ Cifukwa ca ici Ayuda ananimanga ine mu tempele nofunu kunipaya. ²² Mulungu anithandiza kufikila manje, so niimilira kupelekela umboni kuli anthu wamba nakuli olemekezeka sipakhani iliyonse koma zamene aneneri na Mose anakamba zizacitika, ²³ kuti Kristu afunika kubvutika, ndipo azankhala oyamba kuuka kwa kufa kuti alalikile laiti kuli Ayuda na Akunja." ²⁴ Pamene Paulo anasiliza kuzidifenda, Fesitasi anakamba mopunda, Paulo, ndiwe ofuntha; pamphunziro yako yakufunthisa." ²⁵ Koma Paulo anakamba ati, sindine ofuntha, olemekezeka Fesitasi; koma molimbika nikamba mau ya zoona namaganizo yali bwino bwino. ²⁶ Cifukwa mfumu iziba pali izi zinthu; ndiponso nikamba momasuka kwa yeve, cifukwa nilinaco cisimikizo kuti kulibe pali izi zili zobisika kuli yeve; cifukwa izi sizina citike mobisika. ²⁷ Mukhulupilira aneneri, Mfumu Agiripa? Niziba kuti mukhulupilira." ²⁸ Agiripa anakamba kwa Paulo, "Pakanthawi kocepa ufuna kuti unikoke nonipanga kunkhala mu Kristu?" ²⁹ Paulo anakamba ati, "Nipemphela kwa Mulungu, kuti ngankhale pakanthawi kocepa kapena nthawi itali, osati imwe cabe, koma onse amene anibvela lero, mungankhale monga ine, koma osati akapolo monga ine." ³⁰ Pamene apo Mfumu inaimilila, na govana, na Benisi, nabaja bamene enze anankhala nabo; ³¹ pamene anacoka mu holo, anakambisa nokamba ati, "Uyu munthu kulibe camene wacita kuti afe kapena kunkhala mujele." ³² Agiripa anakamba ati kuli Fesitasi, "Uyu munthu sembe anamasuliwa ngati sanapeleke nkhanu kwa Siza."

Chapter 27

¹ Pamene tinagwilizana kuti tiyende ku Itali, anaika Paulo naba kaidi enangu mumanja ya msilikali zina lake Juliyasi wakugula ya Ogasitana. ² Tinakwela boti kucoka ku Adaramitiyamu, yamene yenzofunika kupitila ku mbala kwa Asia. So tinayenda ku mumana. Arisitakasi waku Thesalonika ku Masedoniya anyenda na ise. ³ Siku yokokhapo tinafika mu tauni ya Sidoni, kwamene Juliyasi anamusunga bwino Paulo nomulola kuyenda kuli anzake kuti amusamalile. ⁴ Kucoka apo, tinayenda kumumana noyenda muzungulila pa malo ya Sipurasi kwamene kuchingilizwa ku mphembo, cifukwa mphembo yenzo bwela kuli ise. ⁵ Pamene tinatauka manzi yali pafupi Silisiya na Pamfiliya, tinafika ku Mira, tauni ya Lisia. ⁶ Kuja, msilikali anapeza ciboti cikulu kucokela ku Alekizandiriya yamene yenzo yenda ku Itali. Anatifaka mwamene muja. ⁷ Pamene tinayenda pang'ono pang'ono masiku yambili mpaka tinafika muvutikila pafupi na Sinidasi, sitinayende futi ija njila cifukwa mphepo inali ikulu, so tinayenda kupitila pafupi na Keleti, kumbali kwina kwa Salimoni. ⁸ Tinapitila kuja kumbali mobvutikila, paka tinafika pa malo inangu yoitaniwa Feya Havenzi, yamene yalipafupi na tauni ya Lasi. ⁹ Tinatenga nthawi Itali, na nthawi yosala kudya ya Ayuda inapita, ndipo cenzeli cobvuta kuyenda. So Paulo anabacenjeza, nokamba ati, ¹⁰ "Amuna, niwona kuti ngati tizayenda manje, tizankhala ocitika notaya zinthu, osati cabe katundu na boti ikulu, koma myioyo yathu." ¹¹ Koma msilikali anasamalila abosi namwine wake wa boti kupambana zamene anakamba Paulo. ¹² Cifukwa sizenze cotheka kukhala pa haba nthawi ya mphepo, ambili enze paulendo anabauza kuti acokepo, kuti ngati nicokwanisika tingafike ku tauni ya Fonikisi, kuti tikankhale kuja nthawi ya mphepo. Fonikisi ni haba ya Kereti, nakuti iyanga kummawa naku mmazulo. ¹³ Pamene mphepo yakumazulo inayamba kubwela pang'ono pang'ono, aulendo anaganiza benze nazamene benzo funa. Anafaka visimbi vikulu mumazi noyenda ku Kereti, pafupi kumbali mwa manzi. ¹⁴ Pamene panapita nthawi ing'ono ciphepo cikulu cangozi, cochedwa Ulosilidoni, cinabwela na mphabvu kucokela ku Kereti. ¹⁵ Pamene cimphepo cikulu cinamenya kusogolo kwa boti namphamvu kuti sitingayende pasogolo, tinagonjela nocikonkelela. ¹⁶ Tana thabila kwamene kwenzelibe mphepo maningi kumbali ya malo yang'ono yocedwa Kauda; ndipo mobvutikila tinakwanisa kupeza tuma boti tung'ono tung'ono. ¹⁷ Pamene anaikenesa mukati, anasebenzesa nthambo zake kumanga ku boti ikulu. Anankhala namantha kuti tithabile mumbali mwa mumana wa Siritisi, so anamasula visimbi vikulu ndipo boti inakokhamo. ¹⁸ Tinabvutika maningi na mphepo, so siku yokokhapo benze paulendo banayamba kucosa katundu mu boti. ¹⁹ Siku yacitatu anayamba kuponya cothandizila boti namanja yawo. ²⁰ Pamene zuba na nyenyezi sizinaoneke sizina wale pali kwa masiku yambili, ndipo cimphepo cikulu kumenya ku boti, ciyembekezo cinasila. ²¹ Pamene anankhala nanjala nthawi Itali, pamene apo Paulo ananyamuka pakati pawo nokamba ati, "Azibambo, simbe mwenze munanibvelela, sembe sitinacoke ku Kereti kuti tipezeke mugosi nakutaya katundu." ²² Mannje nikulimbikisani kuti tilimbikile cifukwa kulibe moyo uzataika pakati paimwe, koma cabe kuonengeka kwa boti ikulu. ²⁴ Cifukwa usiku wasila mngelo wa Mulungu wamene nitumikila, wamene nilambila -angelo wake anaimilila pafupi na ine ²³ nokamba ati, "Osayopa, Paulo. Uzaimilila pamaso pa Siza, ndipo ona, Mulungu muchifundo cake wakupasa onse amene uyenda nawo. ²⁵ Cifukwa caici, azibambo, limbikilani, cifukwa nikhululupilira Mulungu, kuti zizacitika monga mwamene anani uzila. ²⁶ Koma mphepo izatikankila pambali. ²⁷ Pamene masiku yali 14 yanasila, pamene mphepo inatikankila uku na uku mu Cimumana ca Adiriyatiki, pakati pa usiku enze paulendo anaganiza kuti enzofika poyuma. ²⁸ Anatenga copimila kutalimpha kwa manzi ndipo anapeza kuti yenze 40 mitazi, panapita nthawi ing'ono, anapima futi ndipo anapeza kuti yenzeli 15 mitazi. ²⁹ Anayopa kuti angamenye kumwala, so anaika visimbi vikulu vili 4 mumazi ndipo anapemphela kuti kuce mwamusanga. ³⁰ Baja benze paulendo enzo sakila njila yocokelamo mu boti ndipo anacosa tumaboti tung'ono kutufaka mumazi, noganizila kuti azaponya visimbi kusogolo kwa boti. ³¹ Koma Paulo anakamba ati kuli msilikali na asilikali, pokhapo ngati aba anthu ankhalilira mu boti ikulu, suzapulumuka. ³² Ndipo asilikali anajuba nthambo za boti noilekela kuti iyende. ³³ Pamene kwenzo kuca, Paulo analimbikisa onse kuti adye cakudya. Anakamba ati, "Lero nisiku ya 14 yamene muyembekeza ndipo simukudya; kulibe camene mwadya. ³⁴ So nikupemphani mudyu vakudya, cifukwa ici cili pankhukhala na moyo wanu; ndipo kulibe coipa cizacitika kwa imwe." ³⁵ Pamene anakamba izi, anatenga buredi noyamika Mulungu pamenso ya aliyense. Ndipo ananyema buredi noyamba kudya. ³⁶ Pamene apo bonse analimbikisika nakudya vakudya. ³⁷ Tenzeli banthu 276 mu boti ikulu. ³⁸ Pamene anadya mokwanila, banapesusa boti pakucosamo tiligu noyitala mumana. ³⁹ Pamene nunabwela kwacha, sanzibe pamene enzeli, koma anaona poyuma, ndipo banakambila ngati bangayendepo na boti. ⁴⁰ So banajuba vinsimbi novitaila mu mana. Pantawi yamene ija banajuba nthambo zacidirayivilo nonyamula cinyula capasogolo pa boti kuli mphepo; ndipo anayenda ku mbali kwa manzi. ⁴¹ Koma banafika pamalo pamene mimana ibili yakumana, ndipo boti inayenda pansi. Ndipo pansi kusogolo kwa boti kunajama nokanga kuyenda, koma kumbuyo kwa boti kunayamba ku tyoka cifukwa cacimphepo cikulu. ⁴² Maganizo ya asilikali yenze yakuti apaye

akaidi kuti pasankale nangu amozi amene azanyaya nothaba.⁴³ Koma mu silikali anafuna kupulumusa Paulo, so anabalesa kucita vamene enzo nganiza kucita; ndipo analamulila kuti baja bamene aziba kunyaya ba jumpe poyamba noyenda poyuma.⁴⁴ Ndipo bonse osalila bakonkhe pambuyo, benangu benzeli pama pulanga, benangu pazinthu zinangu kucoka mu boti. Munjila iyi cinacitika kuti bonse tinafika bwino poyuma.

Chapter 28

¹ Pamene tinafika bwino, tinamvela ati penzo itaniwa kuti Mata. ² Banthu bakwamene kuja, sibanankale babwino cabe, koma banatiyashila mulilo notilandila bonse, cifukwa ca mvula na mphepo yamene siyenzoleka. ³ Koma pamene Paulo anatenga tukhuni notufaka pa mulilo, njoka inacoka cifukwa camulilo, nomuluma Paulo nokangamila kukwanja kwake. ⁴ Pamene banthu bakuja banaona njoka kucoka kukwanja kwake, anakambisana, "Uyu munthu zoona niwopaya wamene anathaba kucoka ku mumana, koma sanaloledwe kuti ankhale namoyo. ⁵ So anakukhumulira njoka ija pamulilo ndipo sinalumiwe. ⁶ Benzo yembezela kuti avimbe cifukwa columiwa nanjoka kapena kumwalila. Koma pamene anayembekezela panthawi nowona kuit kulibe cinacitka codabwisa, banasintha maganizo nokamba ati enze ka mulungu. ⁷ Manje pafupi penzeli malo yenze ya afumu ya baja malo, zina lake Pubiliyasi. Anatilandila ndipo antipasa zofunikala kwa masiku ya tatu. ⁸ Cinacitika kuti atate bake ba Pubiliyasi anadwala mphepo namumala mwa kamwazi. Pamene Paulo anayenda kuliyeve, anamu pemphelela, nomuyika manja pali yeve, nomucilisa. ⁹ Pamene ivi vinacitika ivi, banthu bonse paja pamalo benze odwala anabwela ndipo anacilisidwa. ¹⁰ Banthu banatilemekeza nazinthu zambili. Pamene tenzokonzekela kuyambapo, banatipasa zamene tenzofuna. ¹¹ Pamene panapita mwezi itatu, tinanyamuka mu boti yaku Alezandiriya bamene benze anasiya nthawi ya mphepo, wamene mutu wake wenze mubale wake. ¹² Pamene anafika mu tauni ya Sirakozi, ninakhalako masiku yatatu. ¹³ Kucoka paja tinayenda nofika ku tauni ya Regiyamu. Pamene panapita siku imozi mphepo yaku mazulo inanyamuka, ndipo mumasiku yabili tanafika ku tauni ya Puteoli. ¹⁴ Kuja tinapeza abale ndipo banatiitana kuti timkhale nabeve masiku yali 7. Kucokaka apo tinayenda ku Romu. ¹⁵ Kucoka paja abale, pamene anamvela za ise, anabwela kukumana nase benangu kucoka ku Mariketi ya Apiyasi naku 3 Taveni. Pamene Apulo anabona abale, anayamika mulungu ndipo analimbikisiwa. ¹⁶ Pamene anangena mu Romu, Paulo anavomelezewa kunkhala yeka na msilikali wamene enzo mugandig'a. ¹⁷ Ndipo cinacitika kuti patapita masiku yatatu Paulo anaitana pamozi baja banthu benzeli asogoleli pakati pa Ayuda. Pamene anabwela pamozi, anakamba ati kwa beve, "Abale, ngankhale kuti sininapange mulandu kubanthu or mwambo wa atate bathu, ninapelekewa ngati kaidi kucoka ku Yelusalemu kupelekewa mumanja ya ya Aroma. ¹⁸ Pamene bananifunsa, banafuna kunimasula, cifukwa kwenzelibe cifukwa kuti nipaiwe. ¹⁹ Koma apmene Ayuda anakamba kusushana zofuna yeve, bananipansa kukamba na Siza, ngakhale kuti sicenzeni monga nenzo leta mulandu kuli calo canga. ²⁰ Cifukwa cakupeleka mulandu kwanga, ndiye apo, napempha kuti nikuwone nokamba naiwe. Nificukwa cakuti Israyeli ali naco ciyembezo cakuti ndine omangiwa muma cheni aya." ²¹ Ndipo anakamba ati kwa yeve, Sitinalandile ma kalata kucokela ku Yudeya pali iwe, kapena abale aliwonse anabwela norepota kapena kukamba ciliconse coipa pali iwe. ²² Koma tifuna timvele kuli iwe camene uganiza pali aka ka gulu, cifukwa nocoizibika kuli ise kuti pali ponse bakambapo zoipa pali keve." ²³ Pamene banamufakila siku, banthu bambilianabwela kuli yeve monga malo yopumulilapo. Anapeleka nkhanu kuli beve, nopelekela umboni pali ufumu wa Mulungu. Anayesa kubakonjesa pali Yesu, bonse ba lamulo ya Mose nawocokela ku aneneri, kucoka kuseni paka mumazulo. ²⁴ Benangu anagonjela pazinthu zamene zinakambiwa, koma benangu sibanakhulupilire. ²⁵ Pamene sibanagwilizane beka-beka, banacoka pamene Paulo anakamba aya mau amozi, "Mzimu Oyela anakamba bwino pali Yesaya mneneri kuli makolo banu. ²⁶ Anakamba ati, 'Yenda kuli aba banthu nokamba ati, Pankhani yomvela muzamvela koma simumvesesa, Ndipo kuwona muzaona koma simuzaonesesa. ²⁷ Cifukwa mitima ya aba banthu yankhala yoyuma, Matu yawo yanamvela movutika, banavala menso yawo; kuti basawone na menso yawo, nomvela na matu yawo, novesesa na mitima yawo, notembenuka, ndipo ningabacilise." ²⁸ Cifukwa ca ici, mufunika kuziba kuti ici cipulumuso ca Mulungu cinapelekewa kuli Akunja, ndipo azavela. ²⁹ (Ndipo pamene anakamba izi zinthu Ayuda anacokapo. Kweze kusushana ku kulu pakati pawo.) ³⁰ Paulo anankhala zaka zibili munyumba yamene analenting'a yeka, ndipo analandila bonse bamene anamuyendela. ³¹ Enzo lalikila ufumu wa Mulungu ndipo enzo phunzisa zithu pali Ambuye Yesu Kristu mopanda mantha. Kulibe anamulesa.

Romans

Chapter 1

¹ Paulo, kapolo wa Yesu Khristu, oitanidwa kunkhala mtumiki, opatulika ku uthenga wa Mulungu. ² Uyu ndiye uthenga wamene analonjeza kudala kupitira mubaneneli na malemba olera. ³ Uyu uthenga niwa mwana wake

wamene anabadwa mu banja la Davide kulingana na thupi. ⁴ Kupitila mukuukisidwa kwa akufa, Anamuika kunkhala mwana wa Mulungu wa mphamvu kupitila mu muzimu wa chiyero -Yesu Christu Abuye watu. ⁵ Kupitila muli eve talandila chisomo na utumiki kamba ka kumvela kwa chikhulupililo pakati pamaiko onse, kamba ka zina yake. ⁶ Pakati pa aya maiko naimwe mwaitaniwa kunkhala ba Yesu Christu. ⁷ Iyi kalata niyaonse ali ku Roma, okondewa na Mulungu, oitanidwa kunkhala banthu oyera. Chisomo chinkhale naimwe, namtendere kuchokela kwa Mulungu atate wathu na ambuye Yesu Christu. ⁸ Choyamba niyamika Mulungu kupitila mwa Yesu Christu chifukwa cha imwe monse. Chifukwa chikhulupililo chanu chalalikiwa kuziko yonse. ⁹ Pakuti Mulungu wamene nitumikila nimboni yanga, mumuzimu wanga, mu uthenga wa mwana wake, mwamene nimakambila pali imwe nthawi zambili. ¹⁰ Nimapempha nthawi zonse mumapemphelo kuti munjila iliyonse kuti pothela nizakwanilisa mwachifunilo cha Mulungu kuti nibwele kuli imwe. ¹¹ Pakuti nifunisisa kumuonani, kuti nikamupaseni mphaso ya uzimu, kuti nikamulimbikiseni. ¹² kutanthauza kuti nifunisisa ku kulimbikisidwa pamozi naimwe. kupitila mu chikhulupililo cha wina na mzake, imwe naine. ¹³ Manje sinifuna kuti munkhale osaziba abale, kuti nthawi zonse nenalikufuna kubwela kuli imwe (koma ninalesewa kufikila manje), kuti nikakololepo pali imwe, monga mwamene nakololapo pakati pa akunja. ¹⁴ Ndine wankhongole kuli Agiliki nabenangu bobwela kuchokela kwina, kuli ba nzelu nabalibe nzelu. ¹⁵ Ine nili okonzeka kulalikila uthenga kuli naimwe muli ku Roma. ¹⁶ Pakuti sinichita manyazi na uthenga, chifukwa ndiye mphamvu ya Mulungu ku chipulumuso kwa aliyense okhulupilila, kuyambila Ayuda nama Giliki. ¹⁷ Chifukwa mwamene umo chiyelo cha Mulungu chivumbulusiwa kuchokela kuchikhulupililo kufikila ku chikhulupilo, monga mwamene chinalembewa kuti 'olungama azankala na umoyo mwa chikhulupililo.' ¹⁸ Pakuti mkwiyo wa Mulungu wavumbulusiwa kuchokela kumwamba kwa onse alibe umulungu na onse alibe chiyelo, amene posoba chiyelo abweza kumbuyo choonadi. ¹⁹ Ichi nichifukwa chakuti chija chamene chizibika pali Mulungu nichoonekela kwabeve. Chifukwa Mulungu wabaunikila. ²⁰ Pakuti zozibika zake zamene sizioneka, zamene ni mphamvu zake zamuyaya na mwamene alili kulingana na umulungu wake, zaonekelatu po onekela, kuchokela pamene ziko lapansi inapangiwa, muvinthu vamene vinapangiwa. palibe angakambe kuti sininazibe. ²¹ Ichi ni chifukwa chakuti, banazibako vinthu pali Mulungu, sibanamukweze monga mulungu kapena kumuyamika. Koma banankhala opusa mumaganizo yao ndipo mitima yao ilibe nzelu inankala namudima. ²² Banazona kuti nibanzelu koma banakhala opusa. ²³ Banachinjanisa ulemelelo wa Mulungu wamene siungaonongeke na vinthu vamene vionongeka va umunthu, nyoni, vinyama vamendo yanai na nyama zokwaba. ²⁴ Mulungu anabalekelela kuti bachite zolalakala zao kulingana namutima wao, kuti mathupi yao yankhale yosebanyika pakati pao. ²⁵ Nibeve bana chinjanisa choonadi cha Mulungu na boza, ndipo banapembeza chilengedwe mumalo mopembeza mulungu, wamene alambiliwa kwamuyayaya, Amen. ²⁶ Kamba ka ichi Mulungu anabapasa kuzilakolako zosayenela, chifukwa bazimai babo banachinjanisa zilakolako zabo na vamene vishusana na chilengedwe cha umunthu. ²⁷ Chimozi mozi amuna nao anasiya zilakolako zao na azimai nakuyamba ku kufunana beka beka bamuna. Aba benze bamuna bamene banachita zonyansa na bamuna banzao nakulandila chilango pazonyansa banachita. ²⁸ Chifukwa sibanavomeleze maganizo ya Mulungu mu nzelu zabo, anabapeleka kunzelu zopusa, kuti bachite vinthu vosayenela. ²⁹ Banazuliwa nauchimo wina uliwonse, zoipa, kunkala kwa uchimo, maganizo yoipa. Niwozuliwa na zokumbwila, ndewo, chinyengo, namaganizo yoipa. ³⁰ Nibamijedo, okamba zoipa pabanzao, nakuzonda Mulungu. Niba chiwawa, bantota, nakuzitukumula. Ndiye bamayamba voipa vonse, sibamvelela makolo babo. ³¹ Balibe kumvesesa, siungabakulupilile, balibe zilakolako zaumunthu, balibe chifundo. ³² Bayaziba malamulo ya Mulungu, kuti bamene bachita ivi bafunika kufa. Koma sibachita chabe ivi veka koma bavomekeza nabamene bavichita.

Chapter 2

¹ Siuzapasiwa mpata iwe munthu wamene uweluzwa,chifukwa chamene uweluzwa muli wina naiwe uzaweluziwa.Pakuti iwe wamene uweluzwa uchita vimozi mozi. ² Koma tiziba kuti chiweluzo cha Mulungu chilingana na zoona chikagwela pali bamene bavichita ivi vinthu. ³ Koma ona ichi iwe munthu, wokonda kuweluzwa banthu bamene bachita ivi olo kuti naiwe uchita vimozi .Nanga uzauthaba chiweluzo cha Mulungu? ⁴ kapena uganza pangono pazaulemelelo waubwino wake,chilango chake chamene kucedwa kwa chilango chake,na kuleza mtima kwake?Siuziba kuti ubwino wake ufanika kukupeleka kukulapa? ⁵ Koma nikamba ka kulimba mtima nakusalapa kwa mtima wanu kuti,kuti muzisungila mweka mkwiyo pasiku ya mkwiyo,ndiye kuti,siku ya chivumbuluso cha chiweluzo cha Mulungu choyera. ⁶ Azalipila muthu aliyense muyeso wazinthu zamene anachita. ⁷ Kuli awo olingana na kupitiliza,zochita zabwino,afuna funa kubapembeza,kubalemekeza nakubapasa umoyo wosatha ulibe chiphuphu. ⁸ Koma kuli baja wofuna chabe zao,bamene sibamnvelela chazoon koma amnvelela uchimo,mkwiyo nakukalipa kopitilila kwamene kuzabwela. ⁹ Mulungu azaleta mabvuto na kusamnvelela bwino pa moyo uliwonse wamene wachita chimo,kuyambila kwa Ayuda na ba Giliki. ¹⁰ Koma chiyamiko,ulemu na mtendere vizabwela kuli aliyense wamene achita vabwino.Kwa Ayuda nama Giliki onse.Chifukwa kulibe kusankha kwa Mulungu. ¹¹ Koma kubambili bamene banachimwa kulibe lamulo,bazaonongeka futi kulibe lamulo. ¹² Bambili bazachimwa naulemu wa lamulo,bazaweluziwa na lamulo. ¹³ Pakuti sibaja womnvelela lamulo oyera pamenso pa Mulungu,koma ochita lamulo ndiye bamene bazalungamisiwa. ¹⁴ Pakuti akunja,bamene balibe lamulo,bachita mwaumunthu vinthu va lamulo,bankala lamulo kwabeve beka,olo kuti balibe lamulo. ¹⁵ Pali ivi bawonesa kuti machitidwe yofunika na lamulo niyolembeka mumitima yao.Chikumbumtima chao chichitila umboni kuli beve,namaganizo yao yabanamizila kapena yabachingiliza kuli beve na kuli Mulungu. ¹⁶ Icho chizachitika pasiku yamene Mulungu azaweluzwa visinsi vabanthu onse,kulingana na uthenga wanga,kupitila mwa Yesu Christu. ¹⁷ Koma ngati uziitana muyuda,upumulila pa lamulo nakuzitukumulila mwa Mulungu, ¹⁸ Ndipo aziba chifunilo chake,nakuziba zinthu zabwino chifukwa munapasiwa zochita kuchokela ku lamulo. ¹⁹ Ngati musimikizikila kuti ndimwe osogolela osayangana,nyali kulibaja bali mumdim. ²⁰ Osogolela opusa,mphunzisi wa bana bangono,nakuti mulinacho mumalamulo,nzeli na choonadi,nanga ichi chimukhuzani bwanji mwamene munkhalila umoyo wanu? ²¹ Imwe bamene muphunzisa benangu,simuziphunzisa?Imwe bamene mumalalikila kuti osaiba,mumaiba? ²² Imwe bamene mukamba kuti osachita chigololo,mumachita chigololo?Imwe bamene muzonda mafano,mumaba mu chechi? ²³ Imwe bamene mumasangalala mumalamulo,simumalekeza Mulungu kupitila mukupwanya lamulo yanu? ²⁴ Pakuti zina ya Mulungu siilemekezeka pakati ka akunja kamba ka imwe,monga mwamene chinalembeka. ²⁵ Pakuti mdulidwe umakuphindulilani nga mumnvelela lamulo,koma ngati mupwanya lamulo mudulidwe wanu siunkhala mudulidwe. ²⁶ Manje ngati munthu osadulidwa asunga zofunika zalamulo,kusadulidwa kwake sikungankhala kudulidwa?Nanga wamene sali odulidwa mu umunthu sazakususani ngati wasunga lamulo? ²⁷ Ichi nichifukwa chakuti muli nalamulo yolembeka na mdulidwe,koma muyipwanya lamulo. ²⁸ Pakuti simuyuda wamene nimuyuda kunja,monga mwamene mdulidwe wakunja simudulidwe. ²⁹ Koma nimu Yuda amene nimu Yuda mkati,koma mdulidwe niwuja wamumtima,mumuzimu osati mukalata.Chiyamiko cha munthu wotelo sichichokela kubanthe koma kuli Mulungu.

Chapter 3

¹ Nanga kusi yana kwa muyuda kuli kuti? Nanga phindu ya mdulidwe ipati? ² Nichikulu mnjila iliyonse. Choyamba pazonse ayuda analandila chivumbuluso kuchokela kwa Mulungu. ³ Nanga ngati Ayuda benangu benzelibe chikhulupililo? Ninsi kusakhulupilila kwao kuzalenga kukhulupilila kwa Mulungu kunkhala kulibe phindu? ⁴ Chisankhale telo. Koma lekani Mulungu apezake wazooni, olo kuti munthu aliyense niwaboza. Monga mwamene chalembedwa, kuti mukaonekele kunkhala oyera mumau yanu, nakuti mukapambane pamene mukumana na chiweluzo. ⁵ Koma ngati kusalungama kwathu kuonesha kulungama kwa Mulungu. Tingakambe chani? Kodi tizakamba kuti Mulungu si wolungama kuti alete mkwiyo wake pali ise? (Nisebenzesa mkangano wa munthu) ⁶ Chisankhale telo. Ndaba Mulungu azaweluza bwanji ziko lapansi? ⁷ Koma ngati choonadi cha Mulungu kupitila muboza yanga chileta chiyamiko chambili, nanga nichani muniweluzi kunkhala ochimwa? ⁸ Nanga nichani monga mwamene batinamizila kukamba, monga mwamene benangu bavomekeza, tiyeni tichite choipa kuti chabwino chibwele? Chiweluzo pali beve nicholinga. ⁹ Nichani manje? Nanga ise tizichosapo? awe. Chifukwa tinanamizila kudala a yuda nama giliki, onse, kunkhala panso pachimo. ¹⁰ Ichi chilimonga mwamene chinalembeke. Palibe olungama, olo umozi. ¹¹ Palibe wamene amnvesesa. Kulibe wamene afunisira Mulungu. ¹² Aliyense anapita patali. Onse pamozi banankhala balibe phindu. Palibe wamene achita chabwino, palibe olo umozi. ¹³ Pamkosi pao pali monga manda yoseguka. Malilime yao yanama boza. Ululu wanjoka ulipansi pamalilime yao. ¹⁴ Kamwa kao nikozula na matembeleleo na mkwiyo. ¹⁵ Mendo yao yanachidwi kukhesa mwazi. ¹⁶ Chionongeko namabvuto vili munjila yao. ¹⁷ Aba banthu sibanazibe njila yamtendere. ¹⁸ Palibe mantha ya Mulungu pamenso pao. ¹⁹ Manje tiziba kuti chilichonse chamene lamulo ikamba, ikamba kuli baja bali panso pa lamulo. Ichi nichakuti kamwa kalikonse kakavalike, nakuti ziko yonse yapansi ikaweluzidwe na Mulungu. ²⁰ Ichi nikamba kakuti palibe thupi izalungamisiwa na ntchito za lamulo mumenso mwake. Kupitila mulamulo mubwela nzelu zauchimo. ²¹ Koma manje kuchoselako lamulo, chiyelo cha Mulungu chazibika. Chinapelekewa umboni na lamulo na aneneli, ²² Ndiye kuti chiyelo cha Mulungu kupitila muchikhulupililo mwa Yesu Christu kuli baja bokhulupilila. Chifukwa palibe kusiyanisa. ²³ Pakuti onse anachimwa nakupelebele ku ulemelelo wa Mulungu. ²⁴ Ndipo balungamisiwa na chisomo kupitila mu kuomboledwa kuli mwa Yesu Christu. ²⁵ Pakuti Mulungu anapeleka Yesu Christu kunkala oombola kupitila muchikhulupililo mumwazi wake. Anapeleka Yesu kuti akaonesele chilungamo, chifukwa sanaikoko nzelu kumachimo yakumbuyo mukuleza mtima kwake. Ivi vonse vinachitika kuti akaonesele chiyelo chake pa nthawi ino. ²⁶ Ichi chenze telo kuti akaziwonesele olungama, nakuonesela kuti alungamisa aliyense kamba ka chikhulupililo mwa Yesu Christu. ²⁷ Manje kuzitukumula kuli kuti? Kuchosewapo. pambali iti? yazitchito? iyai koma pambali ya chikhulupililo. ²⁸ Tilize ninshi kuti munthu alungamisiwa na chikhulupililo osati nantchito za lamulo. ²⁹ ³⁰ Kapena Mulungu ni Mulungu waba Yuda chabe? Nanga si Mulungu wa akunja futi? koma ngati Mulungu ni umozi, azalungamisa odulidwa na chikhulupililo, na osadulidwa na chikhulupililo. ³¹ Ninshi tichosepo lamulo kupitila muchikhulupililo? Chisankhale telo. Tisungilila lamulo.

Chapter 4

¹ Manje tizakamba chani kuti Abram, atate wathu mwa thupi anapeza? ² Ndaba ngati Abram analungamisiwa nazitchito, asemble alinayo danga yotumbama, koma osati kutumbama mwa Yesu. ³ Chifukwa malemba akamba chani? Abram anakhulupilila Mulungu ndipo chinapasiwa kwa eve chiyelo. ⁴ Manje kuli wamene asebenza, malipilo yake sichaulele, koma chamene chilichake. ⁵ Koma kuli wamene sasebenza koma akhulupilila muli wamene alungamisa osalungama, chikhulupililo chake chiyeseva chiyelo. ⁶ David naye anakamba daliso kuli muntu wamene Mulungu aona oyera kopanda zintchito. ⁷ Anakamba kuti odalisika nibaja bamene mphulupulu zao zinakhululukiwa, amene machimo yao yanaphimbiwa. ⁸ Odalisika niwuja munthu wamene Mulungu sazabelengela machimo yao. ⁹ Manje nishi iyi nidaliso yokambiwa chabe kuli baja bamene niwodulidwa, olo ili nakulosadulidwa? Pakuti tikamba kuti chikhulupililo chinabelengewa kwa Abram ngati chiyero. ¹⁰ Manje chinabelengewa bwanji? pamene Abram anze mumudulidwe, kapena pamene akalibe kudulidwa? Sichinali Mmudulidwe koma mukusadulidwa. ¹¹ Abram analandila chiwoneselo cha mudulidwe. Ichi chenze chisimikizilo chachiyelo cha chikhulupililo chamene anali nacho kudala pamene sanali mumudulidwe. Chochoka muchiwoneselo ichi chinali chakuti anankhala tate wa onse amene anakhulupilila, olo kuti siwodulidwa. ¹² Ichi chitanthauza kuti chiyelo chinabelengewa kwa beve. Ichi futi chitanthauza Abram anankhala tate wa baja wodulidwa osati chabe kuli baja wodulidwa koma nakuli baja wolondola ndondomeko za chikhulupililo cha atate wathu Abram akalibe kudulidwa. ¹³ Pakuti lonjezo kuti Abram nakuli mubadwo wake wamene unafanika kulobela ziko lapansi, sinabwele kamba ka lamulo kupitila muchiyelo cha chikhulupililo. ¹⁴ Ndaba ngati baja bamene bankhala na lamulo bangakhale oloba, nisnhi chikhulupililo chilichabe, ndipo lonjezo ilibe phindu. ¹⁵ Chifukwa lamulo ileta mkwiyo, koma pamene palibe lamulo, palibe kuchimwa. ¹⁶ Mwaichi nimwa chikhulupililo, kuti lonjezo ikapumulile pa chisomo, nakuti ikasimikiziwe kuli mubadwo wa Abram, osati chabe baja bali pansu palamulo koma nakuli bamene bagabana muchikhulupililo cha Abram. Ni tate wa ise tonse. ¹⁷ Monga mwamene nicholembedwa kuti Nakupanga kunkala tate wamaziko yambili. Abram anali pamenso pa uyo wamene anakhulupilila, Mulungu, wamene apasa moyo kuli bakufa nakuitana vinthu vawamene sivilipo monga vilipo kunkhalapo. ¹⁸ Kuchoselako vonse vamaonekedwe yakunja, Abram anakhulupilila Mulungu nachisimikizo cha msogolo. Ndipo anakhala tate wama ziko yambili, kulingana navamene vinakambika, Uzakhala mutundu wako. ¹⁹ Sanafoke muchikhulupililo. Abram anamnvesesa kuti thupi yake sinali kukwanisa kukhala na bana (Chifukwa anali nazaka makhumi khumi) Anazindikila futi kuti sara naye nalingakwanise kubala bana. ²⁰ Koma kamba ka lonjezo ya Mulungu, Abram sananyalanyaze mukusamukhulupilila, koma anapasiwa mphanvu muchikhulupililo nakumuyamika Mulungu. ²¹ Anakhala nacho chisimikizo kuti wamene analonjeza, analinso nayo mphanvu yofikilisa. ²² Motelo naichi chinabelengewa kwa eve monga chiyelo. ²³ Manje sichinalembeke kuti chikaphindulile eve eka, kuti chinabelengeka kwa eve. ²⁴ Chinalembeke futi kwa ise, kwa eve amene chizabelengeka, ise amene tikhulupilila mwa eve wamene anaukisa Yesu mbuye wathu kwa akufa. ²⁵ Uyu ndiye wamene anapelekewa kamba ka mphulupulu zathu ndipo anaukisiwa kutilungamisa ise.

Chapter 5

¹ Pakuti tinayelesewa na chikhulupililo, Tilinawo mtendere mwa Mulungu kupitila mwa Yesu Christu. ² Kupitila mulieve tilinadanga kupitila muchikhulupililo, muchisomo chake tiimilila. Tisangalala na chisimikizo Mulungu atipasa chasogolo, Chisimikizo chakuti tizagabana mu ulemelelo wa Mulungu. ³ Osati chabe ichi, koma tisangalala futi mumasauso yathu. ⁴ Tiziba kuti masauso yabala kupilila, Kupilila kubala kuvomelezewa, ndipo kuvomelezewa kubala chisimikizo cha sogolo lathu. ⁵ Ichi chisimikizo sichitaisa mtima, chifukwa chikondi cha Mulungu chathiliwa mumitima yathu kupitila mu Muzimu Oyera, wamene anapasiwa kuli ise. ⁶ Chifukwa pamene tenze tikali ofoka, panthawi yake Yesu anafela banthu osalungama. ⁷ Pakuti nichovuta kuti umozi afele olungama. Ndiye kuti kapena munthu angafune kufela munthu wabwino. ⁸ Koma Mulungu aonesela chikondi chake kwa ise, chifukwa pamene tenze tikali ochimwa, Yesu anatifela ise. ⁹ Kwambiri manje, lombamba chifukwa tinalungamisiwa na mwazi wake. ¹⁰ Pakuti ngati pamene tenze tikali badani, tinalungamisiwa kwa Mulungu kupitila mu infa ya mwana wake, kupitililapo, pamene talungamisiwa kwa Mulungu, tipulumusiwa na umoyo wake. ¹¹ Osati chabe ichi, koma tisangalala futi mwa Mulungu kupitila muli mbuye wathu Yesu Christu, wamene kupitila mwa eve talandila kulungamisiwa kwa Mulungu. ¹² Kotelo manje, kupitila mu munthu umozi chimo inangena muzioko lapansi, munjila yamene iyi infa inangena kupitila mu chimo. Ndipo infa inasefukila ku banthu onse, chifukwa onse anachimwa. ¹³ Pakuti kufikila pamene lamulo, chimo inali muziko, pakuti palibe kubelengewa kwa chimo ngati palibe lamulo. ¹⁴ Kotelonso, infa inalamulila kuchokela kwa Abram kufikila kwa Mose, ngakhale pali baja bamene sibanachimwe kulingana na kusamnela kwa Adam, wamene alichoonelako cha uyo wamene abwela. ¹⁵ Olo kuti vili telo, mphaso siili monga chimo. Koma ngati kupitila muchimo ya munthu omozi, bambili banafa, chisomo cha mulungu chinachita kwambili kupitila na mphaso na chisomo cha munthu umozi, Yesu Christu, vipaka kuli bambili. ¹⁶ Pakuti mphaso siili monga vochooka muli munthu ochimwa. Chifukwa munjila imozi, chiweluzo chakususiwa chinabwela kamba ka chimo ya munthu umozi. Munjila inangu, mphaso yochokela mukulungamisiwa inabwela pamene bambili banachimwa. ¹⁷ Pakuti ngati kupitila mumachimo ya banthu umozi, infa inalamulila kupitila mu umozi, kwambili futi baja bamene balandila chisomo chambili, na mphaso ya chiyelo izalamulila kupitila mu omuyo wa umozi, Yesu Christu. ¹⁸ Apa manje kupitila muchimo imozi, Banthu onse anasusiwa, motelonso kupitila mumachitidwe ya chiyelo, kunakhala kulungamisiwa kwa umoyo wa banthu bonse. ¹⁹ Kupitila mukusamnela kwa munthu umozi, bambili banankhala ochimwa, futi kupitila mukumnela kwa umozi bambili bapangiwa oyela. ²⁰ Koma lamulo inangemo, kuchitika kuti chimo ipake. Koma chimo inapaka, chisomo chinapakilako. ²¹ Ichi chinachitika kuti mwamene chimo inalamulila mu infa, momwemonso chisomo chikalamulile kupitila mu chiyelo ku umoyo osatha kupitila mwa Yesu Christ mbuye wathu.

Chapter 6

¹ Nanga chizakamba chani?ninshi tipitilize kuchimwa kuti chisomo chipake? ² Chisankhale telo. Ise bamene tinafa,tizankhala bwanji futi muchimo? ³ Nanga simuziba kuti bambili bamene banabatiziwa mwa Yesu Christu, anabatiziwa mu infa yake? ⁴ Tinaikiwa nay,kupitila mu ubatizo mu infa yake.Ivi vinachitika kuti monga mwamene Yesu anaukisiwa kwa akufa,na ulemelelo wa atate,kuti naise tikayende mu umoyo wamanje. ⁵ Chifukwa ngati taphatikizana naye muchifanizilo cha infa,tizaphatikizana naye mukuukisiwa. ⁶ Tiziba ichi,munthu wathu wakudala anapachikiwa,kuchitila kuti ya uchimo ikaonongeke.Ichi chinachitika kuti tisankhale futi akapolo ku chimo. ⁷ Eve wamene anafa anayesedwa oyela na ulemu wa chimo. ⁸ Koma ngati tinafa na Yesu,tikhulupilila kuti tizankhala na eve futi. ⁹ Tiziba kuti Yesu anaukisiwa ku infa,nakuti siwakufa futi.Infa ilibe ulamulilo pali eve. ¹⁰ Kulingana na infa yamene anafa ku chimo,anafa kamozi pa onse.Koma umoyo wamene ankhala,ankhalila Mulungu. ¹¹ Munjila imozi mufanika muziyese bakufa ku chimo,koma ba moyo kwa Mulungu mwa Christu Yesu. ¹² Motelo musalole kuti chimo ilamulile mumathupi yanu kuti musamnvelele zilakolako zake. ¹³ Osapeleka viwalo va thupi yanu ku chimo,kunkhala zida zosebenzesewa ku vinthu vosaenela. Koma zipelekeni kwa Mulungu monga bakufa bamene manje bali namoyo. Pelekani viwalo vanu kwa Mulungu kuti visebenzesewe ku chiyelo. ¹⁴ Musalole chimo kunkhala na ulamulilo pali imwe. Pakuti simuli pansi pa lamulo koma pansi pa chisomo. ¹⁵ Nichani manje?tichimwe kamba kakuti sitili pansi pa lamulo? Koma pansi pa chisomo. Chisankhla telo. ¹⁶ Nanga simuziba kuti kuwamene muzipeleka monga akapolo ndiye wamene munvela,wamene mufanika kumnvela? Ichi nichazooni olo kuti ndimwe akapolo ku chimo yamene ipeleka ku infa, kapena akapolo ku kumnvela kwamene kusogolela ku chiyelo. ¹⁷ Koma chiyamiko kwa Mulungu.pakuti mwenze akapolo ku chimo, koma munamnvelela mumutima ndondomeko ya chiphunziso chamene munalandila. ¹⁸ Mwankhala omasuka ku chimo,mwapangiwa akapolo ba chiyelo. ¹⁹ Nikamba monga munthu kamba ka zofoka zanuMonga mwamene munapelekela mathupi monga akapolo azinthu zonyansa na zoipa, munjila imozi manje, pelekani ziwalo zathupi ngati akapolo ku chiyelo kuyelesedwa. ²⁰ Pakuti pamene mwenze akapolo ba chimo,mwenze omasulidwa ku chiyelo. ²¹ Panthawi ija, nizipaso zabwanji zamene mwenze nazo pazinthu zimumnvesenai nsoni manje. Chifukwa vochoka mwa ivo vinthu ni infa. ²² Koma manje pamene mwamasuka ku uchimo,ndipo mwankhala akapolo ba Mulungu.mulinamphaso yanu yoyelesedwa. Zotulukamo ni umoyo osatha. ²³ Pakuti mphoto yauchimo ni infa,koma mphaso ya Mulungu ni umoyo osasila mwa Yesu Christu mfumu yathu.

Chapter 7

¹ Kapena simuziba abale (Chifukwa nikamba nabanthu bamene baziba lamulo), kuti lamulo ima lamulila muntu umoyo wake onse? ² Pakuti mkazi wokwatiliwa niwomangika na lamulo kuli mwamuna wake pamene akali moyo. Koma ngati mwamuna wake wafa, ankhala omasuka ku lamulo ya chikwati. ³ Kotelo pamene mwamuna wake akali na moyo, ngati ankhala namuna winangu anankhala mkazi wachigololo. Koma ngati mwamuna wake wafa, ankhala omasuka ku lamulo, sankhala wachigololo ngati ankhala na mwamuna winangu. ⁴ Kotelo abale munapangiwa bakufa ku lamulo kupitila muthupi ya Yesu Christu. Ichi chili telo kuti mukaphatikizane kuli wina, ndiye kuti, kuli uja wamene anaukisiwa kwa akufa kuti tikabale zipaso kwa Mulungu. ⁵ Pakuti pamene tenze muthupi, muzilako lako zauchimo, zoukisiidwa na lamulo, zinali pantchito mumathupi athu kubala zipaso za infa. ⁶ Koma lombamba tamasuka ku lamulo. Tinafa kuli chija chamene chinatipanga ukapolo. Ichi chinankhala telo kuti tikatumikile mu umoyo wasopano mumuzimu, osati mukalata yakale. ⁷ Tizakamba chani manje? Ninshi lamulo nichimo payeka? Chisankhale telo, koma sembe sininazibe chimo, kuti sichinali kupitila mu lamulo. chifukwa sembe sininazibe kukhumbwila chamwine pokhapo lamulo yakamba, ⁸ Koma chimo inatenga Mpata kupitila mu lamulo nakuleta chilakolako muli ine. Pakuti kulibe lamulo chimo niyaakufa. ⁹ Panthawi inangu nenze wamoyo kulibe lamulo, koma pamene lamulo inabwela, chimo inankhala na moyo ndipo ninfa. ¹⁰ Lamulo yamene yenzofunika kuleta omoyo inasanduka infa kuli ine ¹¹ Pakuti chimo inankhala na Mpata kupitila mu lamulo nakunama ine. Kupitila mu lamulo inanipaya. ¹² Kotelo lamulo niyoyela, ndipo lamulo niyolungama, niyoyela, ndipo niyabwino. ¹³ Manje ninshi chabwino chinankhala infa kuli ine? Chisankhale telo. Koma chimo kuchitila kuti ikaonekele kuti nichimo, kupitila mu chamene nichabwino, chinabwelesa infa muli ine. Ichi chinachitika kuti kupitila mu lamulo, kuti chimo ikankhale chimo kupitilila malile. ¹⁴ Pakuti tiziba kuti lamulo niyauzimu, koma ine ndine waku thupi. Ninagulisika ku ukapolo wa chimo. ¹⁵ Pakuti chamene nichita, sinimanimnvesesa, chifukwa chamene nifuna kuchita, sinichichita, ndipo chamene nizonda ndiye chamene nichita. ¹⁶ Koma ngati nichita chamene sinifuna kuchita, nigwilizana na lamulo kuti lamulo niyabwino. ¹⁷ Koma manje sindine wamene achichita ichi, koma chimo yamene inkhala muli ine. ¹⁸ Pakuti niziba kuti muli ine, ndiye kuti mu thupi yanga, mulibe chabwino. Chilakolako cha zinthu zabwino chilimo muli ine, koma sinikwanisa kuchichita. ¹⁹ Pakuti chabwino chamene niifuna sinichita, koma choipa chamene sinifuna kuchita, ndiye chamene nichita. ²⁰ Manje ngati nichita chamene sinifuna kuchita, ninshi sindine nichichita, koma chimo yamene inkhala muli ine. ²¹ Nipeza kansu lamulo muli ine kuti nifuna kuchita chabwino, koma choipa ndiye chili muli ine. ²² Pakuti nisangalala na lamulo ya Mulungu na munthu wamkati, ²³ Koma niwona chinthu chosiyana muziwalo za thupi yanga. Chimenyana na ichi chinthu chanyawane munzeli zanga. Chinisunga ukapolo na nkhanu ya uchimo muziwalo zathupi yanga. ²⁴ Ndine munthu obvutisidwa, ndani azanimasulako ku infa yathupi? ²⁵ Koma tiona Mulungu kupitila mwa Yesu Christu mfumu yathu. Kotelo ine nitumikila lamulo ya Mulungu na nzeli zanga. Koma na thupi yanga nitumikila mphanvu yauchimo.

Chapter 8

¹ Kulibe manje kususiwa kwa baja bali mwa Yesu Christu. ² Pakuti lamulo ya muzimu ya umoyo mwa Yesu Christu yanimasula ku mphanvu ya chimo na infa. ³ Chifukwa chamene lamulo sinakwanise chifukwa inalibe mphanvu kupitila muthupi, Mulungu anakwanisa. Anatuma mwana wake uchimo muchifanizilo cha uchimo wa munthu, kunkhala chopeleka ku chimo, anasusa chimo muthupi. ⁴ Anachita ichi kuti, zofunika za lamulo zikwanilisike muli ise,ise bamene sitiyenda kulingana na thupi, koma kulingana na muzimu. ⁵ Baja bamene bankhala kulingana na thupi,bayika nzelu ku zinthu zakuthupi, koma baja bamene bankhala kulingana na muzimu, baika nzelu kuzinthu zaku uzimu. ⁶ Pakuti kuika nzelu pazathupi ni infa.koma kuika nzelu kuzinthu zaku uzimu niumoyo namtendere. ⁷ Kuika nzelu pazinthu zakuthupi nimkwiyo kwa Mulungu.chifukwa sichigonjela ku lamulo ya Mulungu,ndipo sichikwanisa kuchita telo. ⁸ Baja bamene bali muthupi sibangamukondwelese Mulungu. ⁹ Koma imwe simuli muthupi koma mumuzimu, Ngati nizoona kuti muzimu wa Mulungu unkhala muli imwe.koma ngati mutnu alibe muzimu wa Christu, ninshi siali wake. ¹⁰ Koma ngati Yesu ali muli imwe,ninshi thupi niyakufa ku chimo, koma muzimu ali namoyo kuchiyelo. ¹¹ Ngati muzimu wamene anausa Yesu Christu ankhala muli imwe, uja wamene anausa Christu ku infa azapasa futi moyo kumathupi yanu kupitila mu muzimu wamene akhala muli imwe. ¹² Manje abale na imwe bankhongole,koma kuthupi kunkhala monga baku thupi. ¹³ Chifukwa ngati munkhala kulingana na thupi, mulipafupi nakufa, koma ngati mwauzimu,mupaya zochitika za thupi, muzankhala na moyo. ¹⁴ Koma onse bamene basogololewa na muzimu nibana ba Mulungu. ¹⁵ Pakuti simunalandile muzimu waukapolo kuti munvele mantha. Munalandila muzimu wakutengewa monga bana, muli eve tilila kuti Aba Tate. ¹⁶ Muzimu uchitila umboni na muzimu wathu kuti ndise bana ba Mulungu. ¹⁷ Ngati ndise bana, ndise futi oloba,oloba ba Mulungu. Ndipo ndise oloba na Yesu, ngati tivutika naye kuti tikakwezedwe futi na eve. ¹⁸ Chifukwa niona kuti mabvuto yamene tipitamo manje siyangalingane na ulemelelo wamene uzabvumbulusiwa wa ise. ¹⁹ Pakuti chiyembekezelo chakuya chachilengedwe chiyembekezela chivumbuluso cha bana ba Mulungu. ²⁰ Pakuti chilengedwe chinawoneka kuti chilibe phindu, osati kuchifunilo chake, koma kwa uja wamene anachiwonesela. ²¹ Nichisinsi chosimikizika, kuti chilengedwe chamene chizamasulidwe ku ukapolo ku kuola, nakuti chizabwelesedwa ku ufulu wa ulemelelo wa bana ba Mulungu. ²² Tiziba kuti chilengedwe chonse chibuula,nakusebenza mukubaba pamozi kufikila manje. ²³ Osati chabe ichi, koma naife bamene,tilinazo zipaso za Muzimu, naise tibuula mkati mwa ise, kuyembekeza kutengewa monga bana, kupulumusidwa kwa mathupi yathu. ²⁴ Kamba ka chisimikizilo ichi tinapulusiwa, pakuti chamene tisikizila chizachitika chikalibe kuwoneka, nanga nindani wamene ayembekezela chinthu chamene waona kudala. ²⁵ Koma ngati tilinacho chisimikizo cha vinthu vamene tikalibe kuona, tichiyembekeza moleza mtima. ²⁶ Munjila imozi muzimu atithandiza muzofoka zathu.Pakuti sitiziba mopemphelela,koma muzimu amatipemphelela na kubuula kwa kuya. ²⁷ Wame asecha mitima azaiba maganizo ya muzimu, chifukwa apemphelela okhulupilika kulingana na chifunilo cha Mulungu. ²⁸ Tiziba kuti baja bamene bakonda Mulungu,vinthu vonse visebenzela pamozi ku ubwino wao,Baja oitanidwa kulingana na chifunilo cha Mulungu. ²⁹ Chifukwa bamene anaziba, anabakonzela sogolo kuti akalingane na chifanizilo cha mwana wake.kuti akankhale mwana oyamba pali abale bake bambili. ³⁰ Baja bamene anaizibilatu sogolo yao,aba anabaitana, Baja bamene anaitana, anabalungamisa, Bamene analungamisa anabakwezeka. ³¹ Nanga tizakamba chani pali ivi vinthu?Ngati Mulungu alikumbali yathu nindani angatisuse? ³² Eve wamene sanachite kaso na mwana wake koma anamupeleka kwa ife tonse,nanga azaleka bwanji kutipasa zonse zamene tifuna? ³³ Nindani azabwelesa kususa bana ba Mulungu? Mulungu ndiye wamene amalungamisa. ³⁴ Nindani azatisusa? Yesu ndiye wamene anatifela,kupitililapo anaukisidwa.Alamulila na Mulungu pa malo yaulemelelo.ndipo niyeve atipemphelela ise. ³⁵ Nindani azatilekanisa ku chikondi cha Mulungu?Manzunzo,zovutisa,zobaba,njala,usiwa,koyofyewa kapena lupanga? ³⁶ Monga mwamene chinalembedwa,kuti imwe mukaphindule tipaiwa siku lonse,tingewa monga nkhusa zamene ziyenda kupaiwa. ³⁷ Muvonse ivi tichila baja bopambana, kupitila muli wamene anatikonda, ³⁸ Pakuti nilinacho chisimikizo kuti, ngakhale infa, kapena umoyo, angelo, maulamulilo, vinthu vamanje, kapena vinthu vakusogolo, kapena mphanvu, ³⁹ mwamba kapena pansu, kapena chinthu chinangu chilichonse cholengedwa chizalekanisa ku chikondi cha Mulungu, chamene chili muli Yesu Christu mfumu yathu.

Chapter 9

¹ Nimuuzani vazooni muli Christu, sininama, ndipo chikumbumtima chinichitila umboni mu muzimu woyela ² kuti kuli ine pali manzunzo yambili, nakubaba kosasila mumutima wanga. ³ Ningafune kuti ine wamene nitembeleleke nakupatulika kwa Yesu kamba ka abale banga, baja bamutundu wanga kulingana naku thupi. ⁴ Niba israeli. Bali na cholowa, ulemelelo, na vipangano, mphaso zalamulo, chipembezo cha Mulungu namalonjezano. ⁵ Bawo nimakolo kwamene Yesu anachokela kulingana nakuthupi. eve wamene ali Mulungu pa vonse. iye ayamikike kwa muyayaya. Amen. ⁶ Koma sikuti malonjezano ya Mulungu yakangiwa. Sialiyense mu israeli wamene nimu israeli vazooni. ⁷ olo mubadwo wa Abram siwonse bana ba Abram vazooni. Koma nikupitila muli Isaac kuti bana banu bazaitanidwa. ⁸ Ndiye kuti, Bana baku thupi sibana ba Mulungu. Koma bana ba lonjezo bayesedwa mkoka. ⁹ Pakuti aya nima ya lonjezo. Panthawi iyi nizabwela, ndipo mwana mwamuna azapasiwa kuli Sarah. ¹⁰ Osati chabe ichi, Pamene Rabeka naye atankhala na pathupi kupitila mu munthu umozi, atate bathu Isaac- ¹¹ chifukwa bana benze bakalibe kubadwa, ndipo benze bakalibe kuchitapo chilichonse chabwino kapena choipa. kuti chilingo cha Mulungu kulingana nakusankha kunkhazikike. osati kamba ka zichitidwe, koma kamba ka uja oitana. ¹² Chinakambiwa kuli eve 'Mkulu azatumikila mufana' ¹³ Nichoyenela monga mwamene chinalembewa "Yokobo ninakonda koma Esau ninazonda." ¹⁴ Tizakamba chani manje? Ninshi kulibe chiyelo kwa Mulungu? Chisankhala telo. ¹⁵ Pakuti anati kwa Mose, Nizankhala na chifundo pa wamene nizachitila chifundo. ndipo nizachita chikondi pa wamene nizachitila chikondi. ¹⁶ Kotelo sikuli uja wamene afuna, kapena kuli uja wamene ahamanga, koma kuli Mulungu wamene aonesha chifundo. ¹⁷ Pakuti malemba yakamba kuli Pharaoh, pachilingo chamene ichi ninakunyamula, kuti nikaonesele mphanvu zanga muli iwe, nakuti zina yanga ikalalikiwe muziko yonse ya pansi. ¹⁸ Kotelo Mulungu amachitila chifundo pa munthu wamene afuna. Na wamene afuna amulimbisa Mtima. ¹⁹ Muzakamba kuli ine, Nichani akali kupeza cholakwa? Nanga nindani angakangane na chifunilo chake? ²⁰ Kumbali kwinangu, munthu ndiwe ndani wamene uyankhana na Mulungu? Nanga cholengedwa chingakambe na olenga "Nanga nichani unanipanga tele?" ²¹ Nanga oumba alibe danga youmba kuchokela kudothi imozi kuumba butiza yosebenzesa panthawi yapadela na butiza yosebenzesa siku iliyonse? ²² Nanga ngati Mulungu wamene ali ofuna, kuonesa mkwiyo wake nakuonesa mphanvu yake, anapilila nakuleza mtima mabutiza ya mkwiyo yokonzekela chiwonongeko? ²³ Nanga ngati anachita ichi kuti akaonesele kulemba kwa ulemelelo wake, pama bitiza ya chifundo, yamene ankonza kudala ku ulemelelo wake? ²⁴ Nanga ngati anachita ichi futi kuli ise amene anitana osati chabe kuchokela kwa Ayuda, koma kuchokela nakuli akunja? ²⁵ Monga mwamene akambila mu Hoseya, Nizaitana banthu banga bamene sibanali banthu banga, ndipo wokondedwa wake wamene sanali okondedwa. ²⁶ kotelo chizankhala kuti, pamene chinakambika kuli beve'sindimwe banthu banga' Bazaitaniwa bana ba Mulungu wamoyo. ²⁷ Esaya afuula pali israeli, olo kuti bana ba israeli banali bambili monga michenga yakunyanja, Baja bazasala ndiye bazapululumuka. ²⁸ Pakuti Mulungu azapeleka chiweluzo chake paziko lapansi, kosilizilatu mosanyalanyaza. ²⁹ Monga mwamene Esaya anakamba kudala, kuti Mulungu wamakhamu sanatisile bana, sembe tenze monga sodoma, sembe tinankhala monga Gomola. ³⁰ Tizakamba chani manje? Kuti akunja amene sanali kulondola chiyelo, analandila chiyelo, chiyelo mwa chikhulupilo. ³¹ Koma israeli wamene anafunafuna lamulo yachiyelo, sanafikepo. ³² Nanga chani? Chifukwa sanachilondole na chikhulupililo, koma na ntchito. Banakhumudwa pamwala okhumudwapo, ³³ Monga mwamene chalembeza "onani nizaika mwala mu zion, mwala wamulandu. Wamene azakhulupilila sazachitiwa manyazi.

Chapter 10

¹ Abele kufuna kufuna kwa mtima wanga na pempho kwa Mulungu pali beve, chipulumuso chao. ² Pakuti nipelekela umboni kuti banchilakolako cha Mulungu,koma osati kulingana na kuziba. ³ Pakuti sibaziba chiyelo cha Mulungu,koma bafuna kukhazikisa chiyelo chao. Sibanazipeleke kuchiyelo cha Mulungu. ⁴ Pakuti Yesu nichikwanisilo cha lamulo ya chiyelo,kwa aliyense okhulupilila. ⁵ Chifukwa Mose analemba pa chiyelo chamene chichokela ku lamulo. Munthu wamene achita chiyelo cha lamulo azankhala na chiyelo ichi. ⁶ koma chiyelo chamene chichokela ku chikhulupililo chikamba ichi" Osakamba mumtima wanu,' ndani azayenda kumwamba?' (wamene azabwelesa Christu) ⁷ ndipo osakamba kuti nindani azapita kumanda (wamene azabwelesa Yesu ku akufa) ⁸ Koma chikamba chani? Mau yali pafupi na imwe, mkamwa mwanu namu mtima mwanu. ⁹ Ndiye mau ya chikhulupililo yamene tilalikila. Koma ngati nakamwa kanu muzasimikizila kuti Yesu nimfumu nakukhulupilila mumitima yanu kuti Mulungu anamuukisa ku akufa, muzapulumusidwa. ¹⁰ Pakuti namutima munthu akhulupilila kuchiyelo, nakamwa kake asimikizila ku chipulumuso. ¹¹ Pakuti malemba yakamba kuti, Aliyense wamene akhulupilila mwa eve sazachitiwa manyazi. ¹² Pakuti palibe kusiyana pakti pa Myuda nai mu Giliki.Pakuti mbuye umozi ndi mbuye pa onse, Ndipo niwolemela kwa onse. ¹³ Pakut onse oitanila pali eve azapulumusiwa. ¹⁴ Manje bangaitanile bwanji pali wamene sibanakhulupilile? Bazakhulupilila bwanji wamene sibanamnvelepo? Bazamnvela bwanji ngati palibe mlaliki? ¹⁵ Ndipo bazalalikila bwanji ngati sibanatumiwe? Monga mwamene nicholembewa, Okoma nimendo yabaja bamene banyamula mau yauthenga wabwino. ¹⁶ Koma siwonse anamnvela uthenga,Pakuti Esaya akuti, Mbuye nindani anakhulupilil uthenga wahtu? ¹⁷ Kotelo chikhulupililo chibwela nakumnvela ,ndipo kumnvela mau ya Christu Yesu. ¹⁸ Koma nikamba,nanga sibanamnvele?inde makamaka,Mau yao yapita muziko lonse lapansi,na mau yao kumalekezelo onse aziko. ¹⁹ Kupitililapo nikamba, Israeli sanamnvele?Choyamba Mose akamba kuti 'Nizakuyambani kunjilu' kuwame siziko, Kupitila muziko yosamnvesa, nizaleta kavundula ku mkwiyo. ²⁰ Esaya anali nachisimikizo pakukamba kuti, Ninapezeka nabaja bamene sibananifune. Ninaonekela kuli baja bamene sibananifunse. ²¹ Koma kwa Isreaeli akuti, siku yonse ninapeleka manja yanga ku banthu osamnvela nakuyuma mtima.

Chapter 11

¹ Nikamba ichi, ninshi Mulungu anakana banthu bake? Chisankhale telo. Pakuti naine ndine mu Israeli, mwana wa Abram, wamtundu wa Benajamine. ² Mulungu sanakane banthu bake bamene anaziba kalekale. Kodi simuziba chame malemba yakamba pali Eliya? Mwamene anapapatila Mulungu pali ba Israeli? ³ Ambuye anapaya baneneli banu, banapwanya maguwa, ine neka ndiye nasala, ndipo bafuna kunipaya. ⁴ Koma Mulungu amuyankha chani? Akuti ninasunga banthu wokwanila zikwi khumi ndi ziwili amene salambila mafano. ⁵ Ngakhale telo panthawi ino, kuli baja osala kamba ka kusankha kwa chisomo. ⁶ Koma ngati nimwachisomo, simwantchito. Ndaba chisomo sichizankhala chisomo, ⁷ Nichani manje? Chinthu chamene Israeli anali kufuna, sichinapezeke, koma chosankhiwa chinapezeke, osala banayuma mitima. ⁸ Chilimonga mwamene chinalembewa. Mulungu anabapasa muzimu wopanda nzelu, menso kuti basayangane, namatu kuti basamnvele kufikila lelo. ⁹ Ndipo David anati, lekani tebulo yao inkhale msampha, mwala ochingiliza, nabvuto kwa beve. ¹⁰ Lekani menso yao yachite mdima kuti basaone, nakuti bakhote misana yao kwa muyayaya. ¹¹ Manje nikamba kuti, ninshi banakumudwa kuti bagwe? Chisankhale telo. koma nakukangiwa kwao. Chipulumuso chabwela kuli akunja kuti akabayambe kuchita nsanje. ¹² Ngati kukangiwa kwao nichuma chapaziko, ndipo ngati kutaya kwao nichuma cha akunja, Nanga kusiliza kwao kuzankhala kukulu bwanji? ¹³ Koma manje nikamba naimwe akunja, pokhapo ndine mtumiki kwa akunja, ninyadila utumiki wanga. ¹⁴ Mwina ningachitise nsanje baja bakuthupi ili yanga. Kapena tingapulumuse benangu baiwo. ¹⁵ Ngati kukaniwa kwao kutanthauza kuyanana na ziko, kulandilidwa kwao kuzankhala chani, koma umoyo ku akufa. ¹⁶ Ngati zipaso zoyamba zisungiwa, motelonso choumba cha flao. Ngati mizu zisungiwa, namisambo izasungiwa. ¹⁷ Koma ngati misambo inangu inadukako, ngati imwe, musamba wamsanga wa olive, ngati zinaikiwa mkati mwao, ndipo ngati munagabana nawo mu mizu ya olive yathanzi ya mtengo, ¹⁸ musanyade na misambo. Koma ngati mufuna kunyada, sindimwe mupasa mphamvu ku mizu, koma mizu imupasani mphamvu. ¹⁹ Muzakamba panthawi iyo, Misambo inachokako kuti ine nikaikiwe mkati. ²⁰ Icho nichazooni. Kamba ka kusakhulupilila kwao banadulidwa, koma muimilila nganganga kamba ka chikhulupililo chanu. Musaziganizile kunkhala bapamwamba, koma chitani mantha. ²¹ Pakuti ngati Mulungu sanalekelele misambo ya ku umunthu, naimwe sazamulekelelani. ²² Onani manje, zochita zabwini na kuyopa Mulungu. Mbali imozi, Kuyopa kunabwela pa Ayuda anagwa. Koma mbali inangu, ubwino wa Mulungu ubwela pali imwe, ngati mupitiliza mu ubwino wake. Ndaba naimwe muzadulidwa. ²³ Ndipo nabeve, ngati sibapitiliza mukusakhulupilila kwao, bazaikiwa mkati, Pakuti Mulungu akwanisa kubaika mkati futi. ²⁴ Koma ngati munadulidwa kuchamene mu umuthu, chimtengo cha olive chamsanga, ndipo kususana na umunthu, munaikiwa mu mtengo wa olive wabwino, naga aba Ayuda chizankhala bwanji, amene nimisambo yaku umunthu azabwezewa mu mtengo wao wa olive? ²⁵ Sinifuna kuti imwe musazibe, abale pa chisinsi ichi, kuti musankhale mulibe nzelu mumaganizo yanu. Ichi chisinsi nichakuti kwapezeke kuyuma mutima mu Israeli, kufikila kusiliza kwa Akunja kufike. ²⁶ Ndipo Israeli yonse izapuluma, monga mwamene chinalembewa, kuchokela mu zion kuzankhala muwombolo, Azachosa kusayopa Mulungu konse kuli yakobo, ²⁷ ndipo ichi nichipangano changa nabeve. Pamene nizachosapo machimo yao. ²⁸ Mbali imozi pa uthenga, nibadani banu. Mbali inangu kulingana nakusankha kwa Mulungu, niwokondewa kamba kamakolo yao. ²⁹ Pakuti mphaso namaitanidwe ya Mulungu siyasintha. ³⁰ Pakuti kale simunali kumnvela Mulungu. Koma manje mwalandila chifundo kamba kakusamnvela kwao. ³¹ Munjila imozi, aba ayuda bankhala osamnvela. Chosilizila chinali chakuti kamba ka chifundo chinaonesedwa kwa imwe, nabeve balandile chifundo. ³² Pakuti Mulungu waika onse mukusamnvela, kuti akaonesela chifundo kwa onse. ³³ Kuyendelela kwa chuma cha nzelu zake, nakuziba kwa Mulungu, chiweluzo chake siungachipeze, ndipo njila zake siungazimnvese. ³⁴ Pakuti nindani angazibe maganizo a mfumu kapena ndani anamupasapo nzelu? ³⁵ Kapena nindani anapasapo Mulungu kanthu kalikonse? Kuti Mulungu amubwezele? ³⁶ Chifukwa kuli eve nakupitila muli eve, nakwa eve vonse vintu vilimo. Kuli eve kunkhale ulemelelo kwa nthawi zonse. Amen.

Chapter 12

¹ Nikulimbisani abale kotelo, kulingana na chifundo cha Mulungu, kuti mupeleke mathupi yanu munga nsembe, wachiyelo, olandilidwa kwa Mulungu. Uku ndiye kutumikila kwabwino. ² Musalondole machitidwe yaziko, koma musinhiwe nakunkhala na maganizo yasopano. Chitani ichi kuti muzibe chifunilo. chabwino, cholandilidwa cha Mulungu. ³ Pakuti nikamba kuti kamba ka chisomo chinapasiwa kuli ine, kuti aliyense waimwe asaziwone kuchila munzake, munga mwamene afanika kuganiza. Koma aganize munjila ya nzelu. Munga mwamene Mulungu anapasila muyeso wachikhulupililo kuli aliyense. ⁴ Pakuti tili naziwalo zambili muthupi imozi, koma siwonse alinantchito imozi. ⁵ Munjila imozi, ise tilibambli tili thupi imozi mwa Yesu ndipo payeka payeka ndise membala wa wina ndimzace. ⁶ Tilina mphaso zosiyana siyana kulingana na chisomo chinapasiwa kwa ife. Ngati mphaso yaumozi niuneneli, lekani achite kulingana na muyeso wa chikhulupililo chake. ⁷ Ngati mphaso yawina nikutumikila, lekani atumikile. Ngati winangu alinamphaso yophunzisisa, lekani aphunzisisa. ⁸ Ngati mphaso ya munthu nikulimbikisa, lekani alimbikise. Ngati mphaso yamuthu nikupasa, lekani apase mokondwelesa. Ngati mphaso ya muthu nikusogolela, lekani achite mosamalila. Ngati mphaso ya munthu nikuwonesa chifundo, lekani chite mosangalala. ⁹ Lekani chikondi chinkhale chilibe chinyengo. Kanani choipa, gwilisisani chabwino, ¹⁰ kulingana na chikondi cha abale, nkhalani okondana wina ndi mnzace. Kulingana na ulemu, lemekezanani wina ndi munzake. ¹¹ Kulingana na kusebenzesesa, osanyalanyaza. Kulingana na Muzimu, nkhalani ba chidwi. Kulingana na Ambuye, mutumikileni, ¹² Sangalalani na chisimikizo chamene mulinacho pasogolo lanu. Nkhalani oleza mtima mumabvuto yanu. Pitolizani kupemphela, ¹³ Gabanani muzofuna za okhulupilila, pezani njila zambili zochitilamo zabwino. ¹⁴ Dalisani bamene bamunzunzani, dalisani osatemberela. ¹⁵ Sangalalani nabamene basangalala, Lilani nabamene balila, ¹⁶ nkhalani na nzelu zimozi kuli wina ndi mnzace. Osaganiza munjila yozitukumula, koma landilani bamene bali pansi. Osaziwona banzelu mumaganizo banu. ¹⁷ Osabwezela choipa pa choipa, Chitani zinthu zabwino kuli aliyense. ¹⁸ Ngati nichotheke, makamaka ngati chilipali imwe, nkhalani namtendere na banthu onse. ¹⁹ Osabwezela choipa pakati panu, okondodwa, koma pasani njila ku mkwiyo wa Mulungu. Pakuti nicholembedwa, kubwezela nikwanga, nizabwezela, atelo ambuye, ²⁰ koma ngati mnzako ali nanjala, mudyese, ngati amnvela njota, mupaseni chakumwa, ngati muchita ichi, muzaika makala yamoto pamutu pake. ²¹ Osagonjesewa na choipa, koma gonjesani choipa na chabwino.

Chapter 13

¹ Lekani munthu aliyense ankhale omnvelela mausogolelei yapamwamba. Pakuti palibe usogoleli koma wamene uchokela kwa Mulungu. Mausogolelei onse yamene yaliko yanasankhiwa na Mulungu. ² Mwaichi wamene ashusa maulamulilo aya asusana na ulamulilo wa Mulungu. Ndipo onse osusana na maulamulilo aya azalandila chiweluzo cha Mulungu pali beve. ³ Pakuti asogoleli sasusana na ntchito zabwino, koma zintchito zoipa. Kodi mufunisisa kusayopa baja bali mu usogoli? Chitani zabwino ndipo muzalandila kuvomelezewa kwake. ⁴ Chifukwa nikapolo wa Mulungu kwa imwe kuzinthu zabwino. Koma ngati muchita zoipa, chitani mantha. Pakuti sanyamula lupanga mwachabe. Pakuti nikapolo wa Mulungu, obwezela mukwiyo kuwochita choipa. ⁵ Motelo mumnvelele, osati chabe kamba ka mkwiyo, koma kamba ka chikumbu mtima. ⁶ Kamba ka ichi mulipila ndalama ku boma. Pakuti asogoleli nibatumiki ba Mulungu, bamene bachita ivi vinthu mosaleka. ⁷ Lipilani kuli aliyense nkhangole zamene muli nazo. Ndalama kuwamene afunika kulipiliwa. Nkhangole kuwamene ayenela. Mantha kuwamene tifunika kuyopa, ulemu kuwamene ayenela ulemu. ⁸ Osankhala na nkhangole na aliyense, koma kondanani wina ndimu nzache, Pakuti wamene akonda mnzake akwanilisa lamulo, ⁹ Malamulo, Musachite chigololo, osapha, osaba, osakhumba, ndipo ngati pali lamulo iliyonse, zonse zipezeka mumau aya "Konda mnzako monga mwamene uzikondela wamwine. ¹⁰ Chikondi sichichita choipa ku mnzako, chikondi nichikwaniliso cha lamulo. ¹¹ Kamba ka ichi muziba nthawi, kuti yakwana kudala yakuti muuke kutulo, Chifukwa manje chipulumuso chilipafupi kuchila nthawi yamene tinakhulupilila, ¹² mdima wafika ndipo siku ya yandikila, tsono tiyeni tiyike kumbali ntchito zamumtima, ndipo tiyeni tibvale zida zakuunika. ¹³ Tiyeni tiyende moyenela, monga muzuba, osati mumaphwando yamuziko kapena muzolezelesa, ndipo tisayende muzadama, kapena zilakolako zosayenela, osati mukwiyo kapena nsanje, ¹⁴ koma valani Yesu, ndipo musakhutise zakuthupi, kukwanilisa zilakolako zake.

Chapter 14

¹ Landilani aliyense wofoka muchikhulupililo, osaweluza na mkangano. ² Munthu umozi alinachikhulupililo kudya chilichonse, wina wamene niwofoka akudya chabe zamasamba. ³ Wamene akudya vilivonse asapepule wamene sakudya, ndipo wamene sakudya vonse asaweluze wamene akudya vonse. Pakuti Mulungu amulandila. ⁴ Ndiwe ndani wamene uweluzza kapolo wa munthu winangu? Anyamuka nakugwa pali mbuye wake. Koma azampanga kuimilila, pakuti ambuye akwanisa kupanga kuti aimilile. ⁵ Munthu umozi aona kuti siku imozi ipambana inanso. Wina aona masiku onse chimozi mozi. Lekani aliyense akhale nacho chisimikizo mumtima mwake. ⁶ Wamene aona siku ayiyanganila kwa ambuye ndipo iye wakudya adyele mwa ambuye. Chifukwa apeleka mayamiko kwa Mulungu. Iye wamene sakudya, azichosako kudyela kwa Ambuye, naienso ayamika Mulungu. ⁷ Pakuti palibe wamene azinkhalila yeka, kulibe wamene azifela. ⁸ Pakuti ngati tinkhala, tinkhalila ambuye, ngati tikufa, tifela mwa ambuye. Tafa, sitinafe ndise ba ambuye. ⁹ Chifukwa kamba ka ichi Yesu anafa nakuuka futi, kuti akankhale mbuye pa moyo na bamene bali na moyo. ¹⁰ Koma imwe, nichani muweluzza mbale wanu? Ndipo imwe nichani mupepula mbale wanu? Pakuti tonse tizaimilila pampando wa chiweluzo cha Mulungu. ¹¹ Pakuti nicholembedwa, Malinga nili ndi moyo atelo Ambuye, kwa ine bondo lililonse lizagwada, ndipo lilime iliyonse izapasa mayamiko kwa Mulungu. ¹² Kotelo ndipo aliyense apeleka ndondomeko ya umoyo wake kwa Mulungu. ¹³ Kotelo, tisaweluzane wina ndi mnzake, koma muganize ichi, kulibe wamene azikila chipysinjo kapena msampha ku mbale wake. ¹⁴ ¹⁵ Niziba ndipo nilinacho chisimikizo mwa Yesu Christu, kulibe chinthu chodesedwa pacheka, wamene aona chinthu kuti nichodesedwa, kwa iye nichodesedwa. Ngati kamba ka mwazi mbale wako akhumudwa, ninshi simuyenda muchikondi. Musaononge chakudya chamunthu wamene Yesu anafela. ¹⁶ Musalole chinthu chabwino kuti wina akambe kuti nichoipa. ¹⁷ Pakuti ufumu wa Mulungu sikudya na kumwa, koma chiyelo, mtendere na chimwemwe, mumuzimu oyela. ¹⁸ Pakuti wamene atumikila Christ munjila iyi, avomelezedwa na mulungu komanso banthu bamuvomeleza. ¹⁹ Kotelo, tiyeni tifunefune zinthu zobwelesa mtendere na vinthu vawene vizatimangilila pamozi wina ndi mnzake. ²⁰ Osaononga ntchito ya Mulungu ka ka chakudya, vonse vinthu nivoyela, koma nichoipa kwa uja wamene akudya nakukhumudwisa winangu. ²¹ Nichabwino osadya nyama, kapena kumwa vinyu, kapena chilichonse chamene mbale akhumudwa nacho. ²² Chikhulupililo mulinacho chisungeni pakati paimwe na Mulungu, odalisika niwuja wamene sazisusa na zamene avomeleza. ²³ Wamene sakhulupilila aweluzidwa ngati akudya, chifukwa simwachikhulupililo. Ndipo chamene sichichokela ku chikhulupililo nichimo.

Chapter 15

¹ Manje ise tili olimba timnvelele anzathu ofoka, ndipo tisazisangalase. ² Lekani aliyense amnvese bwino mnzake, pali icho chabwino, kuti amulimbikise. ³ Pakuti Yesu sanazimnvese bwino eve eka, koma mwamene chinalembewa, manyozo ya baja banamunyozi yanagwela pali ine. ⁴ Pakuti chamene chinalembewa kudala, chinalembewa kuti ise tilondole, kuti kupitila mukuleza mtima, na chilimbikiso cha malemba, tikankhale nacho chisimikizo. ⁵ Manje Mulungu oleza mtima na chilimbikiso alengese kuti munkhale na nzelu zimozi, kuli wina ndi mnzake kulingana na Yesu Christu. ⁶ Lekani achite ichi kuti na nzelu zimozi kuti muyamike na kamwa kamozi, Mulungu na tate wa mbuye wathu Yesu Christu. ⁷ Motelo landilani wina ndi mnzake, monga mwamene Yesu anamulandilani, kuchiyamiko cha Mulungu. ⁸ Pakuti nikamba kuti Christu anapangiwa kapolo, wa mdulidwe, kamba ka choonadi cha Mulungu. Kutu akasimikizile malonjezo yanapasiwa kuli azitate, ⁹ ndipo kwa akunja, kuulemelelo wa Mulungu muchifundo chake. Chilimonga chinalembewa, motelo nizapeleka mayamiko kwa imwe pakati pa akunja nakuimbila mayamiko ku zina lanu. ¹⁰ Nafuti ikamba kuti, sangalalani imwe akunja nabanthu bake, ¹¹ nafuti yamikani Mulungu, monse imwe akunja, lekani banthu onse bayamike mulungu. ¹² Nafuti Esaya akamba kuti, kuzankhala mkoka wa Jessie, ndipo ndiye azaima nakulamulila pa akunja. Akunja azankhalanacho chisimikizo. ¹³ Lomba lekani Mulungu wahisimikizo akuzleni na chimwemwe chonse na mtendere pakuti mukhulupilila, kuti mukachuluke muchisimikizo, mwa mphamvu ya Muzimu oyera. ¹⁴ Naine nilinacho chisimikizilo pali imwe abale, nilina chisimikizo kuti imwe namwe ndimwe ozula na ubwino, wozula na nzelu, nilinachisimikizo kuti mukwanisa kulimbikisana wina ndi mnzake. ¹⁵ Koma nilemba izi molimba mtima, kumukumbusani kamba ka mphaso inapasiwa kuli ine na Mulungu. ¹⁶ Iyi mphaso inali yakuti ine ninkhale kapolo wa Yesu Christu ku akunja, kuzipeleka monga wansembe ku uthenga wa Mulungu. Nifanuka kuchita ichi kuti chopeleka kwa akunja chikalandilidwe, kusambisiwa na Muzimu oyera. ¹⁷ Motelo kusangalala kwanga kuli mwa Yesu Christu na muvinthu wa Mulungu. ¹⁸ Pakuti sinizakamba chilichonse koma Yesu Christu anakwanilisa kupitila muli ine ku kumvela kwa akunja. Ivi ndiye vinthu vochitika na mau na machitidwe, ¹⁹ mwamphamvu ya chiwoneselo, na zoziziswa, na mphamvu ya Muzimu oyera. Ichi chinankhala telo kuti kuyambila ku yerusalemu, na madela yapafupi, kufika ku illyricum, kuti nikanyamule wonse uthenga wa Yesu Christu. ²⁰ Munjila iyi, kufuna kwanga kwankhala kulalikila uthenga, koma osati kwamene Yesu azibika naine, kuti nisamange pa maziko ya munthu wina. ²¹ Chilimonga chinalembewa, kulibaja bamene mau yake siyanabwele, bazamuona, ndipo bamene sibanamnvele bazaziba. ²² Nainenso zinalipo zolesa kuti nibwele kwa imwe, ²³ koma pali pano nilibe nthawi yonkhala futi mumadela yakuno, ndipo kwazaka zambili, nankhala nifunisisa kubwela kuli imwe. ²⁴ Pamene nizapita ku Spain, nifuna kumuonani popitilapo, nakuti mukanitume imwe munjila yanga, pamene nizankhala na imwe panthawi itali. ²⁵ Koma apa niyenda ku Yerusalemu, kumikila okhulupilila. ²⁶ Pakuti chinali ubwino wa Macedonia na Achia kupeleka ku osauka, pakati pa okhulupilila ali ku Yerusalemu. ²⁷ Inde chinali ku ubwino wao, nibankhongole bao, pakuti ngati akunja agabana muzauzimu zao, naiwonso afunika kuti abatumikile muzakuthupi. ²⁸ Motelo ngati nasiliza ntchito iyi, nakusimikiza kuti balandila vamene vinatengewa, nizayenda ku Spain nakumutandalilani munjila. ²⁹ Niziba kuti nikabwela kuli imwe nizabwela namadaliso mwa yesu ochuluka. ³⁰ Manje nimulimbikisani abale, mwa mbuye Yesu Christu, na chikondi cha muzimu, kuti muvutike naine mumapemphelo kwa Mulungu pali ine. ³¹ Pemphelani kuti nikapulumusawe kulibaja osamnvela, mu ayaudeya nakuti utumiki wanga ukalandilidwe mu Yerusalemu ku okhulupilila, ³² Pemphelani kuti nikabwele kuli imwe muchimwemwe, kupitila muchifunilo cha Mulungu, nakuti pamozi naimwe nikapeze mupumulo. ³³ Mulungu wa mtendere ankhole naimwe monse. Amen.

Chapter 16

¹ Nisimikizila kwa imwe mlongo Phoebe, wamene nimutumiki ku mpingo waku Cenchrea, ² kuti mukamulandile mwa ambuye, muchita ichi moyenela okhulupilila, ndipo muimilile naye muzonse zamene angafuna. Pakuti uyu wamene wankhala waphindu kuli banthu bambili pamozi naine. ³ Mupase moni Priscilla na Aquila, bantchito banzanga mwa Yesu, ⁴ bamene kamba ka omoyo wanga banaika moyo wao chiswe. Nibayamikila, osati chabe ine neka koma mpingo yonse ya ku Akunja. ⁵ Mupeleke moni ku mpingo wamene uli munyumba yao. Mupase moni epaenetus wokondewa wanga wamene, nichipaso choyamba chaku Asiah mwa Christu. ⁶ Mupase moni Maria wamene wasebenzela imwe kwambiri, ⁷ mupaseso moni Andronicus na junias, ba bululu banga komanso bamene ninalki na beve mu ndende. Nibozibika maningi pakati pa banthu ba Mulungu bamene banali mwa Yesu khristu nikalibe kubwera ine. ⁸ Mupase moni Ampliatu, okondedwa wanga mwa ambuye. ⁹ mupase moni Urbanus, wamene tisebenza nayeve mwa ambuye, na Stachys okondedwa wanga. ¹⁰ Mupase moni Apelles osimikizirika mwa khristu. Mupase moni onse bamene ndi ba munyumba ya Aristobulus. ¹¹ Pasani moni Herodion, mu bululu wanga. Mupase moni ba kunyumba ya Narcissus, bamene bali mwa ambuye. ¹² Mupase moni Tryphaena na Tryphosa, bamene basebenza nchito na mphamvu mwa ambuye. pasani moni Persis okondedwa, wamene wasebenza maningi mwa ambuye. ¹³ Mupase moni Rufus, wosankidwa ni ambuye ni amai bake na amai banga. ¹⁴ Pasani moni Asyncritus, Phlegon, Hermes, Patrobas, Hermas, na ba bululu bamene bali nabeve. ¹⁵ Pasani moni Philologus na Julia, Nereus na mulongosi wake na Olympus na onse ba khristu bamene bali nao. ¹⁶ Mupasane moni wina na winango na ma kiss yabwino. Ma church yonse ya khristu yakupasani moni. ¹⁷ Manje nikupempani, ba bululu, kuti muganizire baja banthu bamene baleta chongo na musokonezo. bayenda pasogolo kuchila zinthu zamene munapunzira. Chokani koni kuli beve. ¹⁸ Chifukwa banthu baso sibasebenzera Khristu, koma mimba zao. Chifukwa cha zamene bakamba zabwino na zonyoza banamiza mitima za banthu balibe mulandu. ¹⁹ Chisanzo cha kumvera kwanu chifika kwa aliyese. Nimvera mushe na inu, manje nifuna ati munkale na nzeru maningi pa za mushe, na opanda mulandu pa zinthu zoipa. ²⁰ Mulungu wa mutendere azapwanya satana manje-manje pansi pa mendo yanu. Cisomo cha ambuye Yesu Khristu chinkale na inu nthawi zonse. ²¹ Timothy, wamene ni sebenza nayeve, amupasani moni, na Lucius, Jason na Sosipater, mu bululu wanga. ²² Ine, Tertius, wamene alemba kalata iyi, amupasani moni mwa ambuye. ²³ Gaius, amene anisunga ine na mpingo onse, amupasani moni. Eratus, osunga ndalama mu mzinda, amupasani moni na Quartus na mu bululu wake. (Ma buku yabwino kopambana yalibe mau aya yali mu ndime iyi) [Onani: Aroma 16:20]. ²⁴ "Lekani chisomo cha Ambuye watu Yesu Kristu chinkale naimwe monse. Amen". ²⁵ Manje ulemu unkhale kwa iye wamene apangisa kuti munkhale oimilira kulingana na mau ya mulungu na vamene Yesu analalikira, kulingana na cibvumbulutso cha zinthu zamene zankhala zobisika zaka zambiri, ²⁶ koma manje, zaululika, komanso mu zamene zinalembedwa mu uneneri zinaululika ku maiko onse, kulingana na malamulo ya Mulungu wa nthawi zonse, pa kumvera chikhulupiliro. ²⁷ Kwa Mulungu yeka wa nzeru, kupitira mwa Yesu Khristu, kunkhale ulemelero nthawi zonse. Amen.

1 Corinthians

Chapter 1

¹ Paulo, anaitaniwa na Kristu Yesu kuti ankhale mutumiki kupitila mu chifunilo cha Mulungu, na Sositenis mubale wathu, ² ku mupingo wa Mulungu ku Kolinto, bamene bana yelesewa mwa Kristu Yesu nakuitaniwa kunkhala banthu boyela, pamozi na bonse bamene mumalo yali yonse baitana pa zina ya Ambuye wathu Yesu Kristu, wamene ni Mbuye wabo na wathu. ³ Lekani chisomo na mutendere vinkhale kuli imwe kuchokela kuli Mulungu Tate watu na Ambuye Yesu Kristu. ⁴ Nima peleka nthawi zonse mayamiko kuli Mulungu pa imwe chifukwa cha chisomo cha Mulungu chamene Kristu Yesu anakupasani. ⁵ Anakupangani kunkhala bolemela munjila zonse, muma kambidwe yonse na nzelu zonse, ⁶ munga mwamene umboni pali Kristu una nkhezikisiwa kunkhala wa zoona pakati panu. ⁷ Mwa ichi simupelebeli mpaso ya uzimu pamene mufunisisa moyembekezela kuonekela kwa Ambuye wathu Yesu Kristu. ⁸ Azakulimbisani kufikila posilizila, mwakuti mukankhale balibe kolakwa pasiku ya Ambuye watu Yesu Kristu. ⁹ Mulungu niokululupilika, wamene anakuitanani mu ubwezi wa Mwana wake, Yesu Kristu Mbuye watu. ¹⁰ Manje nikulimbisani, abale, kupitila mu zina ya Ambuye watu Yesu Kristu, kuti muvomelezane, kuti pasankale mukangano pakati panu. Nikulimbisani kuti mugwilizane pamozi

munzeli zimozi na lingo imozi. ¹¹ Chifukwa ninazibisiba poonekela, abale banga, na banthu ba Kloi kuti pali tuma gulu pakati panu. ¹² Nina kamba ichi: Ali onse pakati kanu akamba kuti, "Ine ndine wa Paul," kapena "Ine ndine wa Apolosi," kapena "Ine ndine wa Kefas," kapena "Ine ndine wa Kristu." ¹³ Nanga Yesu niogabikana? Nanga Paulo anapachikiwapo chifukwa chaimwe? Kapena imwe munabatiziwa muzina ya Paulo? ¹⁴ Niyamika Mulungu chifukwa kulibe wamene ninabatiza pakati kaimwe, kuchoselako chabe Klispas na Gayas. ¹⁵ Ichi chenzeli kuti kusankhale ali onse wamene azakamba kuti anabatiziwa muzina yanga. ¹⁶ (Nina batiza futi na ba mu nyumba ya Stefanasi. Kuchoselako aba, siniziba ngati kuli wina wamene ninabatiza ine.) ¹⁷ Chifukwa Kristu sananitume kuti nikabatize koma kuti nikalalikile utenga wabwino - osati na makambidwe yochenjela, kuti mutanda wa Kristu usachosewepo mpavu zake. ¹⁸ Chifukwa uthenga wa mutanda ulibe pindu kuli baja bamene bamwalila. Koma pakati pa bamene Mulungu apulumusa, ni mpavu za Mulungu. ¹⁹ Chifukwa china lembewa, "Nizaononga nzeli za baja ba nzeli. Nizasokoneza kumvesesa kwa banzeli." ²⁰ Nanga munthu wanzeli ali kuti? Wama punzilo alikuti? Wa ndale wamuziko ino alikuti? Nanga Mulungu sanapindamule nzeli za muziko kuzipanga zilibe pindu? ²¹ Pa kuona kuti ziko kupitila mu nzeli zake si-ina zibe Mulungu, china mvesa bwino Mulungu kupitila mu kusapanga nzeli kwa kulalika kupulumusa baja bamene bakulupilila. ²² Chifukwa ba Yuda bafuna volangiza vodabwisa na ba Giliki bafuna nzeli. ²³ Koma tilalikila Kristu opachikiwa, mwala ogwesa ba Yuda nafuti vilibe pindu kuli ba Giliki. ²⁴ Koma kuli baja bamene Mulungu anaitana, ba Yuda naba Giliki, tilalika Kristu kunkala mpavu na nzeli za Mulungu. ²⁵ Chifukwa kusoba nzeli kwa Mulungu kupambana nzeli za banthu, na kufoka kwa Mulungu ni kwa mpavu kupambana mpavu za banthu. ²⁶ Yanganani kuitaniwa kwanu, abale. Sibambili bamene banali banzeli kulingana na maganizo ya banthu. Sibambili bamene banali ba mpavu. Sindimwe bambili bamene muna badwila ku banja yolemekezeka. ²⁷ Koma Mulungu ana sankha vinthu vilibe nzeli va muziko kuti amvese nsoni ba nzeli. Mulungu anasankha vinthu vilibe mpavu muziko kuti amvese nsoni vinthu va mpavu. ²⁸ Mulungu anasanka vamene vili pansu na vonyozewa muziko. Anasankha vinthu voonewa monga vilibe ntchito, kuti vinthu voonewa monga va mtengo kunkhala vilibe ntchito. ²⁹ Anachita ichi kuti kulibe alionse wamene azazitukumula pa menso pa Mulungu. ³⁰ Chifukwa cha vamene Mulungu anachita, imwe manje muli mwa Kristu Yesu, wamene anankhala nzeli kuli ise zochokela kuli Mulungu. Anankala kulungama kwatu, kuyela, na kuombolewa. ³¹ Chifukwa cha ichi, monga malemba yana kamba, "Mulekeni wamene azitukumula, azitukumule mwa Ambuye."

Chapter 2

¹ Pamene ninabwela kuli imwe, abale, sininabwele namakambidwe yokuchenjelesa kapena wanzelu pamene ninali kulalikila va chisinsi pali Mulungu. ² Chifukwa ninaganiza kuti sinizafuna kuziba kalikonse pamene ninali naimwe koma Yesu Kristu, na kupachikiwa kwake. ³ Ninali naimwe mu mukufoka, na mumantha, na mu kunjenjema. ⁴ Na uthenga wanga na ulaliki wanga siwenzeli wosebenzesa mau yokakamiza ya nzelu. Koma, yenzelili na kulangizila kwa Muzimu na mpamvu, ⁵ mwakuti kukulupilila kwanu kusankale mu nzelu za banthu, koma mu mpavu za Mulungu. ⁶ Manje timakamba nzelu pali baja bokula munzelu, koma osati nzelu za muziko, kapema za bolamulila muthawi uno, bamene bakufa. ⁷ Koma, tikamba nzelu za Mulungu zobisika mu choonadi, nzelu zobisika zamene Mulungu anankazikisa kukalibe kunkhala nthawi ku ulemelelo watu. ⁸ Kulibe bolamulila ba nthawi ino anamvesesa, chifukwa aseme bana mvesesa, aseme sibana pachike mfumu ya ulemelelo. ⁹ Koma monga mwamene chinalembewa, "Kulibe linso yamene inaona, kapena kwatu yamene inamvela, kapena mutima wa muntu wamene unaganizapo vamene Mulungu anakonzekela baja bamene bamukonda"- ¹⁰ Koma Mulungu anasokolola ivi vinthu kuli ise kupitila muli Muzimu. Chifukwa Muzimu umasakila vonse, na vinthu vozama va Mulungu. ¹¹ Nanga nindani wamene aziba maganizo ya munthu kuchoselako muzimu wa uja muntu uli muli eve? Chimozi mozi, kulibe wamene aziba vinthu vozama va Mulungu kuchoselako Muzimu wa Mulungu. ¹² Koma ise sitinalandile muzimu wa muziko koma Muzimu wamene uchoka kuli Mulungu, kuti tizibe vinthu va mahala vamene Mulungu anatipasa. ¹³ Sitikamba pali ivi vinthu mu mau yopunzisiwa na nzelu za muntu koma na Muzimu, kumasulila va uzimu kuli banthu ba uzimu. ¹⁴ Munthu wamene saliwa muzimu sanga landile vinthu vamene va Muzimu wa Mulungu, chifukwa vilibe pindu kuli eve. Sangavizibe chifukwa vizindikiliwa mu muzimu. ¹⁵ Wamene ali wa uzimu aza weluza vonse, koma saweluziwa na benangu. ¹⁶ "Nanga nindani wamene angazibe nzelu za Ambuye, kuti amulangize?" Koma ise tili na nzelu za Kristu.

Chapter 3

¹ Ine, abale, ninakangiwa kukamba naimwe monga bantu ba uzimu, koma monga kubanthu ba ku tupi, monga kuli bana bangono mwa Kristu. ² Ninakumwesani mukaka, osati vakudya vokosa, chifukwa simunali bokonzekela; na apa manje sindimwe bokonzekela. ³ Chifukwa mukali mu vathupi. Pamene nsanje na ndeo vipezeka pakati kanu, ndishi simunkala mankhalidwe yolingana na va kuthupi, na kuyenda kulingana na va umuntu? ⁴ Chifukwa ngati umozi akamba kuti, "Ine nikonka Paulo," na winangu akamba kuti, "ine nikonka Apolosi," kansi ndishi sindimwe chabe bantu? ⁵ Nanga Apolosi nindani? Nanga Paulo nindani? Bakapolo bamene kupitila muli beve muna kulupilala, kuli ali onse wamene Ambuye napasa ntchito. ⁶ ninashanga ndipo Apolosi anatilila, koma Mulungu ndiye wamene anavimelesa. ⁷ Mwa ichi, oshanga nangu otilaila alibe phindu. Koma ni Mulungu wamene akulisa. ⁸ Manje uja wamene ashanga na uja wamene atilila niba mozi, ndipo ali yense azalandila malipilo yake kulingana na nanchito zake. ⁹ Pamozi ndise banchito ba Mulungu. ndimwe munda wa Mulungu, chomangiwa na Mulungu. ¹⁰ Kulingana na chisomo chaMulungu chame chinapasiwa kuli ine monga kaswili ozibisisa kumanga, nina ika maziko ndiopo winangu amangapo. Koma munthu aliyense ankhale ochenjela mwamene amangilapo. ¹¹ Pakuti kulibe wamene angaike maziko yenangu kuchosapo yamene yanaikiwa, yemene ni, Yesu Khristu. ¹² Ngati aliyense amanga pa maziko na golide, siliva, myala ya mutengo wapatali, mapulanga, mauzu, kapena ntete, ¹³ ntchito zake zizaonesewa, chifukwa zuba izazisokolola. Chifukwa izasokololewa mu na mulilo. Mulilo uzayesa kulimba kwa ntchito yamene ali onse achita. ¹⁴ Ngati ntchito ya aliyense iimilila, azalandila malipilo; ¹⁵ koma ngati ntchito ya aliyense yanyeka, sazapezapo chilichonse, koma eve azapumulusiwa, monga uja wamene athaba mu mulilo. ¹⁶ Nanga simuziba kuti imwe ndimwe tempele ya Mulungu na kuti Muzimu wa Mulungu unkhala muli imwe ? ¹⁷ Ngati ali onse aononga nyumba ya Mulungu, Mulungu azamuononga uyo muntu. Chifukwa tempele ya Mulungu ni yoyela, naimwe nimwamene mulili. ¹⁸ Osati ali onse aziname eka. Ngati ali onse pakati kanu aganiza kuti ni wa nzelu mu mubadwe uno, lekani ankhale "chipuba" kuti ankale wa nzelu. ¹⁹ Chifukwa nzelu za muziko muno ni zachabe kuli Mulungu. Monga chinalembewa, "Amagwila banzeli mu kuchenjela kwabo." ²⁰ Nafuti, "Ambuye bamaziba kuti kuganiza kwa banzeli nikwa chabe." ²¹ Chifukwa cha ichi, osati ali onse azitukumule mu bantu. Vonse vintu ni vanu, ²² nangu Paulo, kapena Apolosi, kapena Kefasi, kapena ziko, kapena moyo, kapena imfa, kapena vithu vamene vilipo, kapena vinthu vamene vizabwela. Vonse nivanu, ²³ naimwe ndimwe ba Kristu, na Kristu niwa Mulungu.

Chapter 4

¹ Umu ndiye mwamene munthu afunikila kuti yanganila, monga batumiki ba Kristu ndiponso bolanganila vinthu vobisika va mulungu. ² pa ichi nichofunika kuti bolanganila bankhale bokulupilika. ³ Koma kwa ine ni chinthu cing'ono kuti niweruzidwe naimwe olo nabwalo la milandu. Chifukwa nanemwine siniziweruza neka. ⁴ Siniziba kulakwa kwanga kulikonse, koma sinikamba kuti ndine munthu wamene alibe mulandu. Ni mulungu wamene aniweluza. ⁵ Musaweruze pali chilichonse nthawi ikalibe kukwana, pamene Ambuye akalibe kubwela. Azabwelesa kunyanli vonse vobisika vamu mdima kuonesa vamu mtima. Ndipo aliyense azalandila mayamiko kuchokera kuli mulungu. ⁶ Manje, abale, ninaika malamulo aya pali ine neka na Apollos chifukwa cha imwe, kuti muphunzile kuchoka kuli ise tanthauzo ya kukamba kwa kuti, "Musayende kupitilila vonalembewa." Ichi nichakuti kuti musazitukumule wina na mnzake. ⁷ Pakuti ni ndani aona kusiyana kwa iwe na wina? Ni chani chamene ulinacho chamene siunalandile? Ngati unalawalandila mwaulele, nichifukwa chani uzikweza monga simunachite kulandira? ⁸ Mulikudala na vonse vamene mungafune! Ndimwe olemela kudala! Munayamba kulamulira-mweka kulibe naise! Zooni, nenze ofunisira kuti mulamulile, kuti tilamulile naimwe. ⁹ Chifukwa niganiza kuti mulungu atiyika ise batumiki monga owonekela mumzela osilizila, mumndandanda ndipo monga banthu bamene baweruziwa ku imfa. Tankhala votamba ku ziko- kuli angelo, na ku banthu. ¹⁰ Ndise opusa cifukwa cha Khristu, koma ndimwe banzeru muli khristu. Ndise ofoka, koma ndimwe olimba. Ndimwe olemkezeke, koma sindise osalemekezeke. ¹¹ Mpaka ino ola manje ndise banjala na njota, ndise ovala mosauka, timenyewa moipa, ndiponso tilibe nyumba. ¹² Tisebenza molimba, na manja yathu. Pamene tisuliwa, tidalitsa. Pamene tibvutisiwa, tipilira. ¹³ pamene tinyozewa, tikamba namutima wabwino. Tasanduka, na kuoneka monga, vokaniwa va ziko ndipo vanyansi pavinthu vonse, ¹⁴ Sininalembe ivi kuti nikumvetseni nsoni, koma kuti nikulungamiseni monga bana banga bokondewa. ¹⁵ Ndaba nangu muli na makolo 10 000 muli Khristu, mulibe bazitate bambiri. ¹⁶ Chifukwa ninankhala tate wanu muli Yesu Khristu kupitila mu uthenga wabwino. Nikupemphani kuti mukazinikopeleza. ¹⁷ Ndiye chifukwa chake nakutumilani Timothy, mwana wanga okondewa na okulupilika mwa Ambuye. Azakukumbusani njira zanga mwa Khristu, monga mwamene nibapunzisila kulikonse na mu mpingo ulionse. ¹⁸ Manje benangu pali imwe mwankhala ozitukumula, mucita monga sininali kubwera kuli imwe. ¹⁹ Koma nizabwera kuli imwe manje-manje, ngati nicifunilo cha mulungu. Ndipo niza ona osati chabe kukamba kwa ozitukumula, koma nizaona na mphavu zao. ²⁰ Pakuti ufumu wa Mulungu sulii mu kukamba koma mu mphamvu. ²¹ Mufuna chani? Mufuna nibwere kuli imwe na mkwapu kapena na chikondi na mu mzimu ofasa?

Chapter 5

¹ Tinamvela nkani kuti pali chiwele-wele pakati panu, uchiwelewele wamene siumavomelesewa nakuli bantu bamene balibe Mulungu: Mwamuna atenga mukazi waba tate bake. ² Ndimwe ozitukumula! Simuyenela kulila kansi? Mwakuti wamene achita ichi afunika kuchosewepo pakati kanu. ³ Nangu kuti sinilipo muthupi, nilinaimwe mu mumuzimu. Napeleka kudala chiweluzo pali munthu anachita ichi, munga nenzeliko. ⁴ Pamene mukumana muzina ya Ambuye watu Yesu ndiponso ine nili na imwe mu mumuzimu, ndiponso na mphavu ya Ambuye Yesu ilipo, ⁵ Pelekani uyu munthu kuli Satana kuti vaku tupi vionongeke, kuti muzimu wake upulumuke pa siku ya Ambuye. ⁶ Kuzitukumula kwanu sikwabwino. Kansi simuziba kuti totutumisa tungóno tututumisa mukate wonse? ⁷ Zisukeni mweka ku chotupisa chakudala mwakuti munkale mbali ya sopano ya fulaulo, yamene ilibe chotupisa, munga mwamene mulili. Pakuti Kristu Nkhosa ya pasaka watu, anapachikiwa. ⁸ Mwa ici tiyeni tisangalale pasaka, osati na chotupisa chakudala, chotupisa cha mankalidwe yoipa na uchimo. Mwa ichi, tiyeni tisangalale na mukate wamene ulibe chotupisa koma kutipelekana mu va zoona. ⁹ Ninalemba mu kalata yanga kuli imwe kuti musazipezeka na bantu ba chiwelewele. ¹⁰ Sinina tanthauze kuti pabanthu bachiwelewele bamuziko, kapena bozikonda beka, kapena ma kuluku, nangu bopembeza mafano, chifukwa kuzipatula kuli aba muyenela kuchoka muziko. ¹¹ Apa manje nilemba kuli imwe kuti musazipezeka na muntu aliyense wamene aitaniwa kuti mubale koma ankala umoyo wa chiwelewele, kapena ozikonda, kapena opembeza mafano, kapena osasamalila mau, kapena chakolwa, kapena kuluku. Musadye chakudya pamozi na muntu wamankhalidwe aya. ¹² Nanga ningenamo bwanji kuweluzo bantu bali kunja kwa nyumba ya Mulungu? koma, imwe simufunikila kuweluzo baja bantu bali mukati mwa nyumba ya Mulungu? ¹³ Koma Mulungu aweluzo baja bali kunja. "Chosani muntu oipa pakati panu."

Chapter 6

¹ Ngati umozi akangana na muzake, nishi afunika kuyenda ku Koti ya akunja kupambana pamaso pa banthu bo kululupira? ² Kansi simuziba kuti banthu boyera ba Mulungu bazaweluza ziko yapansi? Ngati muzaweluza ziko, simungakwanise kusiliza tunkani twatu tung'ono? ³ Kansi simuziba kuti tizaweluza angelo? Tingaweluze mopambana bwanji vintu va umoyo uno? ⁴ Manje ngati mungaweluze vamene vikhuzana na umoyo wamasiku onse, nicifukwa chani mupeleka milandu kubanhu balibe poimilira mumpingo? ⁵ Nikamba izi kuti mumvele nsoni. Kansi, palibe wanzelu pakati panu wamene angasilize kuyambana pakati pa abale? ⁶ Koma mubale umozi apeleka mubale wake ku khoti-ndipo mucita ici pamenso pa akunja! ⁷ Cifukwa chopelekana milandu wina na mzake ndimwe ogonjesewa kudala. Nichifukwa cha simungavomeleze kuvutika choipa? Chifukwa chani simunga vomele kunamiziwa? ⁸ Koma imwe ndimwe bamene mucita voipa nonama boza, ndipo mucita ivi kuli ba bale banu! ⁹ Kodi simuziba kuti ocimwa sibazakangena mu ufumu wa Mulungu? Musakulupilile maboza. Baciwelewele nabopembeza mafano, bacigololo, bamuna bachiwelewele, baja bamene bamagonana kususana na chilengedwe, ¹⁰ bakawalala, bozikonda, bachakolwa, bonyoza, na ba kuluku-palibe pali aba bamene bazatengako mbali mu ufumu wa Mulungu. ¹¹ Ndiye mwamene benangu munalili koma munasukiwa, muna yelesewa, munalungamisiwa mu zina ya Ambuye Yesu Kristu na Mzimu wa Mulungu. ¹² "Vonse nivovomelezewa kwa ine," koma sivonse vili na phindu. "Vonse nivovomelezewa kwa ine," koma siniza lamuliliwa nachilichonse. ¹³ "Vakudya nivamu mala, na mala niya chakudya," koma Mulungu azaononga vonse. Thupi si inapangiliwe va chiwelewele, koma thupi niya Ambuye, ndipo Ambuye azapasa vofuna va thupi. ¹⁴ Mulungu anausha Ambuye ndiponso azaushanso naise mwa mpavu zake. ¹⁵ Nanga simuziba kuti mathupi yanu nima membala ya Kristu? Nanga ninga tenge bwanji ma membala ya Kristu na kuyapasa kuli wachiwelewele? Chisankale choncho ai! ¹⁶ Nanga simuziba kuti uja wamene azilundika kuli hule ankhala umozi na eve? Monga mwamene mau yakambila, "Babili bazasanduka umozi." ¹⁷ Koma uja wamene azipeleka kuli Ambuye ankala m'zimu umozi na eve." ¹⁸ Thabani uciwelewele! Chimo iliyonse yamene munthu achita ili kunja kwa thupi, koma muntu waciwelewele acimwila thupi yake. ¹⁹ Nanga simuziba kuti thupi yanu ni nyumba ya M'zimu Woyera, wamene ankhala muli imwe, wamene munalandira kucokera kuli Mulungu? Simuziba kuti simuli pa mweka? ²⁰ Imwe munaguliwa na mtengo wapatali. Cifukwa cha ici lemekezani Mulungu na thupi yanu na mumzimu wanu, wamene uli wa Mulungu.

Chapter 7

¹ Kulingana pa vintu vamene munanilembelapo: "nichabwino mwamuna kusagwila mukazi." ² Koma chifukwa chama yeso yochita vintu vambili vachiwelewele, mwamuna ali onse ankale na mukazi wake, na mukazi ali onse ankale na mwamuna wake. ³ Mumuna afunika kupasasa mukazi wake ,danga yogona naye, chimozi-mozi na mukazi kuli mwamuna wake. ⁴ Simukazi wamene ali na ulamulilo pa thupi yake, koma ni mwamuna. Chimozi-mozi, mwamuna alibe ulamulilo pali thupi yake, koma mukazi wake alinao. ⁵ Musakanilane wina na muzake, koma ngati mwagwilizana kwa ka ntawi . Chitani ichi kuti muzipeleke ku ma pempelo. Ndipo mubwele pamozi futi, kuti Satana asakuyeseni chifukwa cha kukangiwa kwa kuzileza kwanu. ⁶ Koma nikamba ivi vintu kuli imwe mopempa osati molamulila. ⁷ Ningafune kuti bonse bankale monga mwamene nilili. Koma ali onse alinayo mpaso yake yochokela kuli Mulungu. Umozi ali na mpaso ya mutundu uyu, na winangu ali na yosiyana. ⁸ Kuli bosakwatiliwa na bofedwa nikamba kuti ni chabwino ngati bankala bosakwatiliwa, monga mwamene nilili. ⁹ Koma ngati sibakwanisa kuzi lesa, ndishi bakwatile. Chifukwa chilibwino kuti bakwatile kuchila kuti akazipya nachilakolako. ¹⁰ kuli bokwatila nipeleka iyi lamulo-osati ine, koma Ambuye-mukazi asachoke kuli mwamuna wake ¹¹ (koma ngati achokako kuli mwamuna wake, ankale osakwatiliwa koma chabe ngati afuna kubwezana na mwamuna wake), na mwamuna asasiye mukazi wake. ¹² Koma kuli bonse nikamba kuti-ine, osati Ambuye-kuti ngati mubale ali onse ali na mukazi wamene siokulupilila, ngati niokutula kunkala naye, asamusiye. ¹³ Ngati mukazi ali na mwamuna wamene sakulupilila, koma niokutula kunkala naye, asamusiye. ¹⁴ Pakuti mwamuna osakulupilila amapatuliwa chifukwa cha mukazi wake, na mukazi osakulupilila apatuliwa chifukwa cha mubale. Asembe si ivi bana banu sembe bankala ba bosayelesewa, koma nibopatuliwa. ¹⁵ Koma ngati bwenzi osakulupilika ayenda, mulekeni aende. Mu vintu monga ivi, mubale kapena mulongo siomangiwa ku volapa vabo. Mulungu anati itana kunkala mu mutendele. ¹⁶ Nanga uziba bwanj, iwe mukazi, kapena ungapulumusa mwamuna wako? kapena uziba bwanj, iwe mwamuna, kuti ungapulumusa mukazi wako? ¹⁷ Koma lekani ali yense ankale umoyo wamene Ambuye banamunkazikila eve, aliyense mwamene Mulungu anamuitanila. Iyi ndiye lamulo yanga muma kachisi yonse. ¹⁸ Nanga ali yense anali odulisiwa pamene anaitaniwa kuti akulupilile? Asayese kuonekela monga osadulisiwa. Nanga kuliko aliyense wamene anali osadulisiwa pamene anaitaniwa kunkala okulupilila? Asankale osadulisiwa. ¹⁹ Chifukwa si kudilisiwa kapena kusadulisiwa kwamene kuli na pindi. Chamene chipindula ni kukonka malamulo ya Mulungu. ²⁰ Ali onse ankhale mu kuitaniwa kwamene anaitaniwa pamene Mulungu anamuitana kuti akulupilile. ²¹ Nanga munali bakapolo pamene Mulungu anakuitanani? Musaikeko nzelu. Koma ngati ngankhale omasuka, osalekelela mwai. ²² Chifukwa wamene aitaniwa na Ambuye kunkala kapolo ni womasuliwa wa Ambuye. Chimozi-mozi, wamene anali omasuka pamene anaitaniwa kuti akulupilile ni kapolo wa Kristu. ²³ Munaguliwa na mutengo, mosavomeleza kuti munkhale bakapolo ba bantu. ²⁴ Abale, mu moyo ulionse wamene aliyense analili pamene anaitaniwa kuti akulupilile, tiyeni tinkale mwamene umo. ²⁵ Kukamba pali baja bosakwatila, nilibe lamulo ili yonse kuchokela kuli Ambuye. Koma nizakamba kuganiza kwanga monga uja wamene, kupitila mu chisomo cha Ambuye, niwokulupilika. ²⁶ Mwa ichi, niganiza kuti chifukwa cha chionongoke chamene chibwela, chilibwino kuti mwamuna ankale mwamene alili. ²⁷ Ndiwe okwatila? Osafuna kusiya chikwati. Ngati sindiwe okwatila, osasakila mukazi. ²⁸ Koma ngati wakwatila, suna chimwe, nauja mukazi osakwatiliwa ngati akwatiliwa, sanachimwe. Koma baja bamene bakwatila bazankhala na vinthu vosiyana-siyana vovuta va muziko, ndipo nifuna kukupulumusani kuli ivi. ²⁹ Koma nikamba ichi, abale, Ntawi ni ifupi. Kuyambila apa, lekani baja bamene bali na bakazi bankhale monga baja bamene balibe. ³⁰ Baja bamene balila bankhale monga sibalila, nabaja bamene basekelela monga baja bamene sibasekelela, ³¹ nabaja bamene bagula monga baja bamene sibankhala nakali konse, nabaja bamene basebenzesa ziko bankale monga baja bamene sibaisebenzesa mofikapo. Chifukwa ziko mwamene ilili ibwela kosilizila. ³² Nifunisisa kuti munkhale bomasuka ku voganiza. Uja osakwatila aganzila pali vinthu va Ambuye, mwamene angabamvesele bwino. ³³ Koma uja okwatila aikila nzelu kuli va muziko, mwamene angamvesele bwino mukazi wake - ³⁴ niogabika. Mukazi osakwatiliwa kapena namwali aikila nzelu ku vintu va Ambuye, mwamene angazisungile oyela mu thupi na mu muzimu. Koma uja okwatiliwa mukazi aganzila pali vintu va muziko, mwamene angamvesele bwino mwamuna wake. ³⁵ Nikamba ichi kuti imwe mupezepo pindu, osati kuti ni ikepo cholesa pali imwe. Nikamba ichi chinthu chifukwa ichi chinthu chili bwino, kuti munkhale bozipeleka kuli Ambuye kulibe cho sokoneza. ³⁶ Koma ngati muntu ali onse aganzila kuti samupasa ulemu mukazi wake wamene anakolobeka-ngati anapita zaka zamene angakwatiliwepo ndipo chifunika kunkala njila yamen iyi-mulekeni achite chamene afuna. Sachimwa. Bakwatilane. ³⁷ Koma ngati ankazikisa mumutima mwake, ngati sali na vomuvutisa koma akwanisa kulesa vofuna vake, kusunga mukazi wake namwali, azachita bwino. ³⁸ Mwa ichi wamene akwatila mukazi wake achita bwino, na uja wamene asankha kuti asamukwatile achita bwino maningi.

³⁹ Mukazi niomangika kuli mwamuna wake nthawi yonse yamene akali na moyo. Koma ngati mwamuna wake amwalila, niwomasulika kukwatila aliyense wamene eve afuna, koma muli Ambuye chabe. ⁴⁰ Koma muku weluza kwanga azankhala okondwela ngati ankala mwamene alili. Ndiponso niganiza kuti nili nao Muzimu wa Mulungu.

Chapter 8

¹ Manje pa vakudya vopelekewa ku mafano-tiziba kuti "tonse tili nazo nzelu." Kuziba kutukumulisa, koma chikondi chimanga. ² Ngati winangu aganiza kuti aziba chinthu, uyo munthu akalibe kuziba mwamene afunikila kuziba. ³ Koma ngati aliyense akonda Mulungu, uyo munthu azibika kuli eve. ⁴ Manje pa nkhanu ya vakudya vopelekewa ku mafano-tiziba kuti "fano mu ziko niyachabe" ndipo "kulibe Mulungu wina koma umozi. ⁵ Nangu kuti tumilungu twina tuliko, kumwamba kapena pansu, monga mwamene kulili tu "milungu" twambili ndiponso tu "mbuye" twambili. ⁶ Koma kuli ise, Kuli chabe umozi Mulungu Atate, kuchokela kuli eve vonse vintu, wamene tinkhalila na moyo, ndiponso umozi Mbuye Yesu, ndiponso kupitila muli eve ise tinkhalako. ⁷ Koma uku kuziba sikuli muli bonse. M'malo mwake, bena banali kupembeza ma fano, ndiponso bakudya chakudya ichi monga nichinthu chamene chinapelekewa ku mafano. Chifukwa cha ichi mitima zabo zi-onongeka chifukwa nibo foka. ⁸ Koma chakudya sichizatipeleka kuli Mulungu. Sindise opanda pache ngati sitikudya, kapena aphindu ngati tikudya, ⁹ Koma samalilani kuti ufulu wanu usankhale chifukwa cha wina ofoka muchikululupilo kuti agwe. ¹⁰ Muganizile kuti kapena winangu akuonani wamene aziba, mukudya chakudya munyumba ya mafano. Kansi mutima wake wofoka si-uzalimbikisiwa kudya vakudya vopelekewa kuma fano? ¹¹ Manje chifukwa cakumvesesa kwanu pavazoonu va tumilungu, uja ofoka, mubale wamene Yesu anafela, aonongeke. ¹² Ndiye kuti, pamene uchimwila mubale wako, kupanga chilonda mutima wake, uchimwila Kristu. ¹³ Mwa ichi, ngati chakudya chikhumudwisa mubale wanga, sinizadya futi nyama, kuti nisapange mubale wanga kuti agwe.

Chapter 9

¹ Nanga ine sindine omasuka? Nanga ine sindine mutumiki? Nanga sininamuone Yesu Ambuye wathu? Nanga imwe sindimwe vochoka va kusebenza kwanga mwa Ambuye? ² Ngati sindine mutumiki kuli bena, kuli imwe ndine mutumiki. Chifukwa ndimwe chosimikizila utumiki wanga mwa Ambuye. ³ Ichi ndiye chi chingilizo changa kuli baja bamene bamani yesa: ⁴ Nanga tilinayo danga ya kudya na kumwa? ⁵ Kansi tilibe dangay zotenga na ise mukazi wamene anakulupilila, monga mwamene banachitila bonse batumiki, na babale ba Ambuye, na Kefas? ⁶ Kapena ni Banabas na ine bamene tifunika kusebenza? ⁷ Nanga nindani wamene amatumikila ntchito yaasilikali kusebenzesa chuma chake? Nanga nindani wamene amashanga munda wa mpesa koma samadyako vipaso vake? Kapena nindani wamene amabetela nyama koma samamwako mukaka wake? ⁸ Nanga nikamba ivi vintu kukonka mpavu za muntu? Nanga lamulo si imakamba ivi? ⁹ Chifukwa chinalembewa mu malamulo ya Mose, "Usamange pa kamwa ng'ombe pamene ikutwa milisi." Nanga ni ng'ombe zamene Mulungu asamalila apa? ¹⁰ Kansi sakamba pali ise? Chinalembewa ise, chifukwa wamene alima munda afunika kulima na chiyembekezo, nauja wamene asepeta afunikila kupepeta mwa chiyembekezo chaku kololako zokolola. ¹¹ Ngati tina shanga vauzimu pakati panu, nanga ni chintu chikulu ngati takolola vakutupi kuli imwe? ¹² Ngati benangu banali na mpavu izi kuli imwe, kansi ise ndishi sitichilapo? Koma sitina chite ichi. Koma tinalimba muvonse kuti tisankhale bobwezela kumbuyo utenga wa Ambuye Kristu. ¹³ Kansi simuziba kuti baja bamene bamatumikila mu nyumba ya Mulungu bamatenga vakudya vabo mu nyumba ya Mulungu? Kansi simuziba kuti baja bamene bamatumikila pa guwa bamagabana vamene vipelekewa pa guwa? ¹⁴ Chimozi-mozi, Ambuye bana uza bonse bamene batumikila utenga wabwino kutenga malipilo yabo kuchokela mu utenga wabwino. ¹⁵ Koma ine sinina sebenzese danga yanga yonse iyi. Futi sinilemba ivi kuti munichitile chili chonse. Chawamapo ine nafa kupambana kuti munthu ali onse anikanile kuzimvela uku. ¹⁶ Chifukwa ngati ine nilalikila uthenga, nilibe mphavu yo zimvela, chifukwa niyenekela kuchita ichi. Soka kuli ine ngati sini lalikila uthenga wabwino! ¹⁷ Chifukwa ngati ine nichita ivi mofuna, nilinayo malipilo. Koma ngati mosafuna, nili nayo ntchito yamene ina pelekewa kwa ine. ¹⁸ Nanga kansi malipilo yanga nichani? Kutu ngati nilalika utenga, ningapeleke utenga mosalipilisa kuti nisasebenzese danga yanga mu utenga. ¹⁹ Ngakale kuti ndine omasuka kuli bonse, ninankala kaopolo kuli bonse, kuti ninga tengeko bambili. ²⁰ Kuli ba Yuda ninankala monga mu Yuda, kuti niba tengeko ba Yuda. Kuli baja bali pansi pa lamulo, ninankala monga baja bamene bali pansi pa lamulo mwakuti nitengeko baja bali pansi pa lamulo. Ninachita ichi ngakale kuti ine paneka sini nali pansi pa lamulo. ²¹ Kuli baja bali pansi pa lamulo, ninankala monga baja bali kunja kwa lamulo, ngakale kuti sininali kunja kwa lamulo ya Mulungu ine, koma pansi pa lamulo ya Kristu. Ninachita ichi kuti nitengeko baja bali kunja kwa lamulo. ²² Kuli bofoka ninankala ofoka, kuti ningatengeko bofoka. Ninankala vintu vonse kuli bantu bonse, kuti ningayese munjila ili yonse kupulumusako benangu. ²³ Nimachita ivi vonse chifukwa cha cha utenga wa bwino, kuti ningatengeko muma daliso yake. ²⁴ Nanga simuziba kuti mu mpikisano bonse botamanga bamatamanga muma sebela, koma ni umozi chabe wamene amalandila malipilo? Mwa ichi tamangani kuti mu landile mpoto. ²⁵ Ali onse otamanga amazi lesa mu vintu vonse. Bamachita ichi kuti balandile ngalawa yamene imaonongeka. ²⁶ Mwa ichi sinima tamanga monga nilibe cholinga kapena kumenyana kuponya ma kofi mu mpepo. ²⁷ Koma nima lamulila tupi yanga kui panga kapolo, kuti pamene nisiliza kulalikila benangu, ine mwine wake nisakaniliwe.

Chapter 10

¹ nifuna kuti muziwe, abale, kuti atate athu onse anali pansu pa makumbi ndipo bonse banapita pa nyanja. ² bonse banabatizidwa mwa mose mu makumbi na munyanja, ³ ndipo bonse banadya chakudya chimozi cha uzimu. bonse ⁴ banamwa chakumwa chimozi cha uzimu. cufukwa banamwa chakumwa cha uzimu kucokera ku mwala wa uzimu wamene unabalandola, ndipo mwala uyo ni yesu khristu. ⁵ koma mulungu sanakondwere nabo bambiri, na matupi yabo yakufa yanataiwa mu chipululu. ⁶ koma ichi chinali chisanzo kwa ife, kotero tisafune zinthu zoipa mwamene banacitira. ⁷ musankhale opembeza mafano, monga mwamene banalili beve. izi ni monga mwamene zinalembedwa, "banthu banankhala pansu kudya na kumwa, na kuimilira kusebela." ⁸ tisachite chigololo, monga benangu bambiri banacitira. pa siku imozi, banthu 23,000 banafa kamba ka ichi. ⁹ tisafake khristu pa mayeselo, monga mwamene bambiri banacitira ndipo banaonongedwa na njoka. ¹⁰ osankhala odandaula, monga mwamene banacitira benangu ndipo banaonongedwa na mungelo wa imfa. ¹¹ manje izi zinthu zinacitika monga citsanzo kwa ife. zinalembedwa kunkhala maphunziso kwa ife- kwa ife amene kusila kwa mibadwo kwatifikila. ¹² manje lekani aliyense amene aganiza kuti nioimilila ankhale osamalira kuti asagwe. ¹³ palibe mayeso yamene yabwera pa inu yomwe niyosazibika bwino ku banthu. mumalo mwake mulungu ni wa chifundo. sazalola kuti muyesedwe kupitilira mphamvu zanu. pa mayeso yaliyonse azakupasani njira yamene mungathabile, kuti mukwanise kupilira. ¹⁴ kotero, okonedwa, thabani ku kupembeza mafano. ¹⁵ nikamba kwa inu ngati banthu bamvesesa, kuti muweruze zamene nikamba. ¹⁶ chikho cha madaliso chamene tidalisa, sikugawana mu magari ya khristu? mukate wamene tigawana, sikugawana mu thupi la khristu? ¹⁷ chifukwa pali mkate umozi wa mkate, ife amene ndife bambiri ndife thupi limozi. timadya mkate umozi pamozi. ¹⁸ onani pa banthu ba isiraeli: baja bamene bakudya nsembe sibatangako mbali pa guwa? ¹⁹ nikamba chani nanga? kuti fano ni chilichonse? kapena kuti chakudya chopasidwa ku mafano ni chilichonse? ²⁰ koma nikamba pa zinthu zamene akunja a mitundu amapereka, kuti bapereka vinthu ivi kwa vibanda osati kwa mulungu. sinifuna kuti imwe mutengeko mbali na vibanda! ²¹ simungamwe chikho cha mulungu na chikho cha vibanda. simungankhale na chiyanjano pa gome la mulungu na pa gome la vibanda. ²² kapena kuyamba ambuye kuti bankhale na nsanje? kodi ndife olimba kucira yeve? ²³ "chilichonse ndi chololedwa," koma sivonse vapindu. "vonse nivololedwa." koma sivonse vamene vilimbisa banthu. ²⁴ pasapezeke munthu amene afuna vabwino vake eka. mumalo mwake aliyense afunile vabwino nzake. ²⁵ mungadye vilivonse vamene vigulisidwa pa msika, popanda kufunsa mafunso ya chikumbu- mtima. ²⁶ chifukwa dziko ni ya ambuye na vonse vili mkati mwake. ²⁷ ngati munthu osakulupilira akuitanani kuti mudye chakudya, ndipo mufuna kuyenda, idyani vilivonse vamene akupasani popanda kufunsa chikumbu- mtima. ²⁸ koma ngati winangu anena kwa inu kuti, "chakudya ichi chachokera ku nsembe ya mukunja," musadyeko. ichi ni chifukwa cha uja wamene wamuuzani, ²⁹ na chifukwa cha chikumbu- mtima. sinikamba chikumbu- mtima chanu, koma cha munthu wina. chifukwa chani ufulu wanga uziweruzidwa na chikumbu- mtima cha wina? ³⁰ ngati nikudya chakudya ni mayamiko, ni chifukwa chani ninyozedwa pa chinthu chamene napereka kudala mayamiko. ³¹ kotero, olo mudye kapena kumwa, kapena chili chonse chamene muchita, chitani zonse ku ulemelero wa mulungu. ³² musankhale na cholakwa kwa ayuda kapena agiliki, kapena ku nyumba ya mulungu. ³³ nimayesa kukondweresa banthu bonse pa zonse. sinifuna kupindula kwanga, koma kwa bonse. nichita izi kuti bapulumutsidwe.

Chapter 11

¹ Nkalani bokopela ine, monga mwamene ine nimakopela Kristu. ² Manje niku tamandani chifukwa mumakumbukila ine mu vintu vonse. Niku tamandani chifukwa mugwililila myambo monga mwamene ine ninapelekela kuli imwe. ³ Manje nifuna imwe mumvesese kuti Kristu ni mutu wa mwamuna ali onse, kuti mwamuna ni mutu wa mukazi, na kuti Mulungu ndiye mutu wa Kristu. ⁴ Mwamuna ali onse wamene apempela kapena anenela na mutu wovalika achosa ulemu ku mutu wake. ⁵ Koma mukazi ali onse wamene apempela kapena anenela na mutu wake osavalikiwa achosa ulemu ku mutu wake. Chifukwa ni chimozi-mozi kuti mutu wake unali ogelewa. ⁶ Chifukwa ngati mukazi sazabisa mutu wake, agele sisi zake zinkale zifupi. Ngati nicha nsoni kuti mukazi ankale na sisi zo gela kapena kuti eve agele sisi mumutu, lekani abise mutu wake. ⁷ Mwamuna asankale na mutu obisika, chifukwa eve ni chitunzi-tunzi na ulemelelo wa Mulungu. Koma mukazi ni ulemelelo wa mwamuna. ⁸ Chifukwa mwamuna sana lengewe kuchokela kuli mukazi. Koma, mukazi analengewa kuchoka kuli mwamuna. ⁹ Chifukwa sikuti mwamuna analengelewa kamba ka mukazi. Koma, mukazi analengelewa mwamuna. ¹⁰ Ichi ndiye chifukwa chake mukazi aenela kunkala na chisonyezo cha ulamulilo pa mutu pake, chifukwa cha bangelo. ¹¹ Mosatayako nzelu, mwa Mbuye, mukazi sali womasuka kuli mwamuna, kapena mwamuna kunkala omasuka kuli mukazi. ¹² Monga mwamene mukazi amachokela kuli mwamuna, chimozi-mozi mwamuna amachokela kuli mukazi. Ndiponso vintu vonse vichokela kuli Mulungu. ¹³ Weluzani pamweka: kansi nichoyenela kuti mukazi akazipempela kuli Mulungu na mutu obisika? ¹⁴ Nanga chilengedwe cheve sichima kupunzisani kuti mwamuna ngati ali na sisi zitali, nicha manyazi kuli eve? ¹⁵ Kansi nanga chilengedwe sichima kupunzisani kuti ngati mukazi ali na sisi zitali, ni ulemelelo wake? Chifukwa sisi zake zina pelekewa kuli eve kuti zinkale chobisilako. ¹⁶ Koma ngati ali onse afuna kushushana pali ichi, ise tilibe munkalidwe wina, ngakale na mipingo za Mulungu. ¹⁷ Koma mu malamulo aya, siniku tamandani. Chifukwa ngati mwabwela pamozi, sichintu chabwino koma choipa. ¹⁸ Chifukwa poyamba, nimvela kuti pamene imwe mubwela pamozi mu mpingo, pali mukangano pakati kanu, ndipo mumbali nikulupilila. ¹⁹ Chifukwa pali na tuma gulu pakati panu, mwakuti baja bamene banavomelesewa bangazibike pakati panu. ²⁰ Chifukwa pamene mukumana, sichkudya chaku mazulo chaba Mbuye chamene mukudya. ²¹ Pamene mukudya, ali onse akudya chakudya chake pamene benangu bakalibe kudya chakudya chabo. Wina ali na njala, na winangu akolewa. ²² Nanga mulibe ma nyumba yakuti mungadye na kumwelamo? Kansi munyozela nyumba ya Mulungu na kusebanya baja bamene balibe kalikonse? Kansi nichani chamene nizakamba kuli imwe? Nikutamandeni? Sinizakutamandani pa ivi! ²³ Chifukwa ine ninalandila kuchoka kuli ba Mbuye vamene ine ninapeleka kuli imwe, kuti ba Mbuye Yesu, usiku wamene banagulisiwa, banatenga mukate. ²⁴ Pamene banapeleka mayamiko, bana gaba mukate nakukamba kuti, "Iyi ndiye thupi yanga, yamene niyanu. Mukazichita ichi kunikumbukila ine." ²⁵ Munjila imozi anatenga gome pambuyo pakudya, nakukamba kuti, "Iyi gome ni pangano ya manje mu magari yanga. Mukazichita chamene ichi ntawi yonse pamene imwe mukumwamo, kukumbikila ine." ²⁶ Chifukwa ntawi ili yonse pamene mukudya uyu mukate na kumwa iyi gome, mulalikila kufa kwa Ambuye kufikila mpaka pamene Azabwela. ²⁷ Ali onse, mwa ichi, wamene akudya mukate kapena kumwa gome ya Ambuye munjila yosayenela azankala olakwa kamba ka thupi na mwazi wa Ambuye. ²⁸ Lekani muntu azi yese eka poyamba, munjila iyi mulekeni adye mukate na kumwa mu gome. ²⁹ Chifukwa eve wamene akudya na kumwa kopanda ku zindikila thupi ya Ambuye akudya na kumwa chiweluzo chake. ³⁰ Ichi ndiye chifukwa chake chamene bambili pakati kanu nibofoka na kudwala, ndiponso benangu pakati panu banagona. ³¹ Koma ngati ise tiziyesa pa ise teka, sitizaweluziwa. ³² Koma ngati ise tiweluziwa na Ambuye, tilangiwa, mwakuti tisa taiwe pamozi na muziko. ³³ Mwa ichi, abale banga, pamene imwe mubwela pamozi kuti mudyeye, lindilanani wina na muzake. ³⁴ Ngati ali onse ali na njala, mulekeni adye kunyumba kwake, kuti ngati mwabwela pamozi sichizankala chiweluzo. Na pali vinangu vamene imwe munanilembela, niza kuonesani vochita ngati nabwela.

Chapter 12

¹ Pa zampasoza uzimu, abale, sinifuna kuti munkale osaziba. ² Muziba imwe pamene Munali akunja banakusobesani pakukupelekani ku mafano yamene siyakamba, kaya mu njila bwanji yamene Munali kusogolelewa nayo. ³ Mwa ici nifuna kuti imwe muzibe kuti kulibe aliyense wamene akamba na Muzimu wa Mulungu angakambe, “Yesu niwo tembeleleka.” Kulibe angakambe kuuti, “Yesu ndiye Mbuye.” Koma ngati ali na Muzimu Woyela. ⁴ Koma kuli mpaso zosiyana-siyana, koma Muzimu umozi. ⁵ Kuli kutumikila kosiyanasiyana, koma Ambuye umozi; ⁶ Ndiponso kuli kusiya-siyana kwa ntchito, koma ni Mulungu umozi wamene asebenza monse-monse. ⁷ Koma kuli aliyense kunapasiwa kuonekela kwa Muzimu kupindulira bonse. ⁸ Kuli umozi kupasiwa na Muzimu mau ya nzelu, ndipo kuli wina mau ya kuziba na Muzimu umozi. ⁹ Kuli wina kupasiwa chikulupiliro na Muzimu umozi, ndipo kuli wina mpaso zopolesa na Muzimu umozi. ¹⁰ Kuli wina kupasiwa ntchito zo dabwiso, ndipo kuli wina uneneli. Kuli wina kupasiwa kukwanilisa kosiyanisana pa mizimu, kuli wina makambidwe ya vitundu vosiya-siyana, ndipo kuli wina kumasulila chikambidwe cha vitundu. ¹¹ Zonse izi ni ntchito za Muzimu umozi-mozi, kupasa mpaso kuli aliyense pa eka, monga eve asankila. ¹² Monga mwamene thupi ilili imozi koma ili na zigawo zambili koma zigawo zones ni mbali za thupi imozi, nichimozi-mozi na Kristu. ¹³ Chifukwa mu Muzimu umozi tonse tinabatiziwa mu thupi imozi, ngakale kuti ni Ayudah kapena Agiliki, akapolo kapena omasuka, ndiponso bonse banalengewa kumwako Muzimu umozi. ¹⁴ Chifukwa thupi si chigawo chimozi, koma vambili. ¹⁵ Ngati kwendo ikamba kuti, “Onani sindine kwanja, sindine mbali ya thupi,” Ici sichingalengese kuti isankale mbali ya thupi. ¹⁶ Ngati kwatu yakamba kuti, “chifukwa ine sindine linso, sindine mali ya thupi, “si-izaleka kunkala mbali ya thupi. Asembe thupi yonse inali linso, nanga mpavu yomvelela inankala kuti? ¹⁷ Ngati thupi yonse yankala kwatu, nanga mpavu yomvelela kununkila izankala kuti? ¹⁸ Koma Mulungu Anaika chiwago cili chonse, imozi ili yonse, mu thupi monga mwamene anafunila. ¹⁹ Koma ngati vonse vinali chigawo chimozi, kansi asembe thupi inankala kuti? ²⁰ Chifukwa cha ici nivi gawo vambili, koma thupi imozi. ²¹ ²⁴ Linso si-ingakambe kuli kwanja kuti, “Nilibe ntchito naiwe.” Kapena mutu kukamba kuli mendo kuti, “Nilibe ntchito naiwe.” Koma vigawo vonse va thupi vamene vioneka monga vilibe mpavu nivofunikila. ²² Koma vigawo vamene timaganizila kuti sivolemekezewa vili na ulemelelo wa mbili. ²³ Koma vigawo watu vo-onekela sivilinazo vofunikila monga vija. Koma Mulungu anaikisa thupi pamozi, kupasa ulemelelo waukulu kuli vigawo vamene vilibe ulemelelo. ²⁵ Anachita chamene ici kuti pasankale kugabikana pathupi, koma kuti vigawo visamalilane wina na muzake mu chikondi chimozi. ²⁶ Mwakuti ngati, gawo imozi ivutika, vigawo vonse vizavutikila pamozi; kapena ngati gawo imozi yalemekezewa, vigawo vonse vizakondwela pamozi. ²⁷ Manje imwe ndimwe thupi ya Kristu koma pa mweka ndimwe chigawo. ²⁸ Ndipo Mulungu anaikisa mu mpingo oyamba batumiki, bokonkapo baneneri, kukonkapo bapunzisi, bochita vodabwisa, kwabwela mpaso zopolesa matenda, bena bopeleka thandizo, baja bamene basebenza ntchito za usogoleri, nabaja bamene bali na makambidwe ya vitundu vosiyana-siyana. ²⁹ Nanga bonse niba tumiki? Nanga bonse niba neneri? Nanga bonse niba punzisi? Nanga bonse bachata ntchito zodabwisa? ³⁰ Nanga bonse bali nazo mpaso zopelesa matenda? Nanga nibonse bakamba malilime? Nanga nibonse bakwanisa kumasulira vikambidwe va vitundu. ³¹ Funisisani mwa changu mpaso zikulu. Koma nizakulangizani njila yabwini maningi.

Chapter 13

¹ Ganizilani kuti ine nikamba na ma lilime ya bantu na ya ba Ngelo. Koma ngati nilibe chikondi, nankala cholinza cha chongo kapena ngoma ya chongo. ² Ganizani kuti nili na mpaso ya uneneli ndipo nizibisisa vonse vintu vobisika na nzelu, ndipo nili na chikulupililo chakuti ninga chonse mapili. Koma ngati ine nlibe chikondi, ine nilibe pindu. ³ Ganizani kuti napasa vonse vamene nili navo kudyesa bosauka, ndipo nipeleka thupi yanga kuti iochewe. Koma ngati nilibe chikondi, sinipindula kali konse. ⁴ Chikondi nichopilila. ⁵ Chikondi sichi kumbwa kapena kuzitukumula. Chilibe ntota kapena kupanda ulemu. Sichiziganizila. Sichimakalipa pafupi-pafupi, kapena kupenga vo chilakwila. ⁶ Sichima kondwela mu vintu vilibe chilungamo. Koma, chimasangalala mu vazo-ona. ⁷ Chikondi chipilila mu vintu vonse, chikulupilila vintu vonse, chiyembekezela vintu vonse, ndiponso chipilila mu vintu vonse. ⁸ Chikondi sichisila. Ngati kuli ma uneneli, yazapita. Ngati kuli ma lilime, yazasila. Ngati kuli nzelu, zizapita. ⁹ Chifukwa ise tiziba tungóno ndiponso tinenela mu mbali. ¹⁰ Koma pamene chofikapo chibwela, chija chamene chili chosafikapo chizapita. ¹¹ Pamene ine ninali mwana, ninali kukamba monga mwana, ninali kuganiza monga kamwana, kuganiza kwanga kunali monga kwa mwana. Pamene ine ninakula, ninasiya vintu va bana. ¹² Chifukwa manje apa tiona mosafikapo monga mu mila, kukonkapo nkope pa nkope. Apa nizibako chabe pangóno, koma paja nizakaziba mofikapo monga mwamene ine nizibilika mofikapo. ¹³ Koma manje ivi vintu vitatu visala: chikulupililo, chiyembekezo, na chikondi. Koma chikulu pali ivi ni chikondi.

Chapter 14

¹ Tamangilani chikondi ndipo mufunisisa mpaso za uzimu, maka-maka kuti mukazinenera. Chifukwa uja wamene akamba malilime sakamba na bantu koma na Mulungu. Chifukwa kulibe ² wamene amumvela ndaba akamba vachisinsi mu Muzimu. Koma ³ wamene anenela akamba ku banthu kubamangilisa, ⁴ kubalimbikisa, na kubathonthoza. Eve wamene akamba mu lilime azimabgilisa eve eka, koma wamene anenera amanga m'mpingo. ⁵ Manje ine ningafunisisa kuti monse mukazikamba mu ma lilime. Koma kuchilapo, ningafunisisa kuti imwe mukazinenera. Eve wamene anenera nimukuru kuchira wamene akamba mu ma lilime (Koma ngati pali omasulira kuti m'mpingo upezapo chilimbikio). ⁶ Koma apa, abale, ngati nabwela kuli mwe nikamba malilime, nizakupindulani chani imwe? Sinizachita, koma ngati nakamba naimwe na chivumbuluso, kapena nzelu, kapena uneneli, kapena chipunziso. ⁷ Chimozi-mozi, ngati vilimba vilibe moyo vichosa mau-monga ka m'tolilo kapena ngoli-ngati sivichosa mau osiyana-siyana, nanga muntu ali-yense azaziba bwanji chamene m'tolilo kapena ngoli ilinza? ⁸ Chifukwa ngati m'tolilo ilinziwa na maimbidwe yamene siyazibika, muntu angazibe bwanji kuti iyi ni ntawi yokonzekela nkondo? ⁹ Nichimozi-mozi iwe na lulimi. Ngati ukamba mau yosamveka bwino, vizamveka bwanji vamene vikambiwa? Uzayamba kukamba na mpepo. ¹⁰ Mosakaikila kuli vitundu vosiyana-siyana pa ziko yapansi, koma kulibe chilibe pindu. ¹¹ Koma ngati siniziba tantauzo ya chitundu nizankala m'kunja kuli wamene akamba, nawamene akamba azankala m'kunja kuli ine. ¹² Niche mozi-mozi naimwe. Chifukwa mufunisisa kuonekesela kwa Muzimu, funisisani kulimbikisiwa kwa mupingo mwakuti munga pake. ¹³ Mwa ici, uja wamene apempera mu lilime aenela kupempela kuti amasulile. ¹⁴ Chifukwa ngati nipempela mu lilime, muzimu wanga upempera, koma nzeru zanga sizitengapo pindu. ¹⁵ Nizachita chani kansi? Nizapempera na muzimu wanga, koma futi nizapempera na nzeru zanga. Nizaimba na muzimu wanga, koma futi niza na nzeru zanga. ¹⁶ Manje ngati sivichitika munjila iyi, ngati wadalisa Mulungu na muzimu, azakwanisa bwanji mukunja kukamba kuti, "Amen" pamene iwe upeleka mayamiko ngati saziba vamene ukamba? ¹⁷ Zoona, upeleka mayamiko mokwana mofikapo, koma uja muntu winangu salimbikisiwa. ¹⁸ Niyamika Mulungu chifukwa nikamba malilime kuchila imwe monse. ¹⁹ Koma mu mpingo ningasankepo kukamba mau yasanu yomveka kuti nipunzise benangu, kuchilapo kukamba mau yali zikwi kumi mulilime. ²⁰ Abale, musankale bana mumaganizo yanu. Koma, pa nkani ya voipa, nkalanu munga bana, koma mumaganizo mwanu nkalanu bakulu. ²¹ Mu lamulo nicholembewa, "Kupitila muli bantu ba malilime yachilendo na milomo za balendo nizakamba nabo aba bantu. Na apa sibazakani mvela," akamba Ambuye. ²² Manje malilime ni chisanzo, osati kuli bo kululupilira, koma kuli bosakululupira, koma uneneri ni chisonyezo osati kuli bokululupilira, koma kuli bokululupilira. ²³ Ngati mupingo wonse wabwela pamozi ndipo bonse bakamba mu malilime, ndipo bakunja na bo sakululupila babwela, kansi sibazakamba kuti ndimwe bosokonezeka? ²⁴ Koma ngati bonse baimwe munenera ndipo osakululupira kapena wakunja abwela, azagwiliwa navimene vikambiwa vonse. Azaweluziwa na vonse vamene vikambiwa. ²⁵ Vobisika va mumutima wake vizafuluka. Chokonkapo azagwa pansu na nkope yake naku pembeza Mulungu nakukamba kuti, Mulungu ali na imwe pakati kanu. ²⁶ Chokonkapo ni chani manje? Abale, pamene mubwela pamozi aliyense ali na nyimbo, chipunziso, chivumbuluso, lilime ngakale kumasulira, chitani vonse kuti mumange mpingo pa mwamba. ²⁷ Ngati winangu pali imwe akamba mu malilime, lekani pankale babili mwina mwake batatu, aliyense mwa ku bwelela, wina amasulile vamene vakambiwa. ²⁸ Koma ngati palibe winangu womasulika lekani bonse bankale chete mu mupingo, lekani aliyense akambe eka kwa Mulungu. ²⁹ Lekani baneneri batatu bakambe, lekani benangu bankale bomvelela pa vimene vikambiwa. ³⁰ Koma ngati pa chivumbuluso kwa uja wamene ali nkale pansu lekani woyamba ankale chete. ³¹ Kuli aliyense anga nenere, mozi-mozi kuti, aliyense apunzile ndikuti onse alimbikisiwe. ³² Muzimu wa muneneri umvelela muneneri. Chifukwa ³³ Mulungu si Mulungu wa musokonezo, koma mtendere. ³⁴ Bakazi bankale chete mu mpingo, chifukwa siwololewa kukamba, afunika, amvesese, munga lamulo ikamba. ³⁵ Ngati pali chintu chamene bafuna ku punzila, afunse bamuna babo ku nyumba; pakuti cipasa manyazi ngati mkazi afunsa mu mpingo. ³⁶ Nanga mau ya Mulungu yanachokela imwe mweka? Ndimwe chabe yanabwewe? Ichi ndiye lamulo mu mpingo yonse ya Mulungu woyela. ³⁷ Ngati aliyense aganiza kuti eve ni muneneri, muntu wa uzimu, aziwe kuti vintu vimene nikamba ni lamulo ya Ambuye. ³⁸ Ngati winangu satizindila ivi, musamuzindikile na eve. ³⁹ Manje abale nifunsisa-Nikufuna, kunerea, musalese aliyense ku Kamba mumalilime, ⁴⁰ Vonse vichitike mwa mtendere musankale namusokonezo.

Chapter 15

¹ Manje nifuna kuzibisa kwa inu, abale, uthenga wamene ninalalikila kwa inu, wamene munalandila nawamene mu imililapo, ² ndipo kupitila mwamene mupulumusidwa, ngati mugwililira mwa mphavu mau yamene ninalalikila kwa imwe, pokhapo munakululupira mwa chabe ³ Ninapeleka kwa imwe ngati chintu chofunikila chamene inenso ninalandila, kuti Yesu anafa kamba ka macimo yathu kulingana na malemba, ⁴ kuti anaikidwa m'manda, ndipo kuti anaukisiidwa pa siku lacityatatu kulingana na malemba. ⁵ Yesu anaonekela kwa Kefasi, ndipo pambuyo pake kuli ali twelovu; ⁶ ndipo anaonekela ku abale opitilila five hundred pa ntawi imozi. Ambiri ba ibo bakali na moyo, koma benangu banagona tulo. ⁷ Ndipo anaonekela kwa Yakobo; pa mbuyo pake kuli batumiki bonse. ⁸ Posilizila pake, anaonekela kwa ine, monga kwa uja munthu anabadwa nthawi isanakwane. ⁹ Ine ndine osilizila pali batumiki. Sindine oyenela kuitaniwa mutumiki chifukwa ninasausa mupingo wa Mulungu. ¹⁰ Koma mwa chisomo cha Mulungu nili mwamene nilili, ndipo chisomo chake chili mwa ine sichinali cha chabe, ninasebenza mwa mphavu kupambana bonse. Koma sindine iyayi, koma chisomo cha Mulungu chili naine. ¹¹ Chifukwa cha ichi angankhale ndine kapena beve, mwamene umo tinalalikila ndipo munakhulipirila. ¹² Manje ngati Yesu alalikiwa monga owukisiwa kwa akufa, nanga nibwanji kuti benangu mwa imwe mukamba kuti kulibe ku ukisiwa kwa akufa? ¹³ Manje ngati kulibe ku ukisiwa kwa akufa ndiye kuti ngankhale Yesu sanaukisiwe; ¹⁴ ndipo ngati Yesu sanaukisiwe ndiyekuti ulaliki wathu uli wacabe, ndipo chikhulupiro canu cili mwa cabe. ¹⁵ Nafuti tipezeka kuti ndise bakamboni baboza pa va Mulungu, chifukwa timapeleka umboni kuti Mulungu ana muukisa Kristu kumchosa ku imfa. Koma ngati sana mu'ukise eve, ngati ni cha zooni kuti bakufa siba ukisiwa. ¹⁶ Koma ngati bakufa sibaukisiwa, nga kale Kristu sanaukisiwe; ¹⁷ ngati Kristu sanaukisiwe, chikululupiro chanu ni cha chabe-chabe, ndipo mukali mu chimo ¹⁸ Ndipo baja bamene banagona tulo mwa Kristu banaonongeka. ¹⁹ Ngati mumoyo uno tili na chiyembekezo mwa Kristu, pa banthu bonse ise timvesa chifundo. ²⁰ Koma manje Kristu, wamene ni oyamba kuli baja bamene banamwalila, anaukisiwa ku bakufa. ²¹ Pakuti imfa inabwela kupitila mu bantu, kupitila mu bantu kunabwela ku ukisiwa kwa bakufa. ²² Pakuti mu Adam bonse bama mwalila, chimozi-mozi mwa Kristu bonse bazapasiwa moyo. ²³ Koma ali onse mu malo yake: Kristu, wamene ni oyamba, kukonkapo bonse bamene niba kwa Kristu bazaukisiwa pa kubwela kwake. ²⁴ Kukonkapo kusiliza, pamene eve azapeleka ufumu kwa Mulungu Atate, pamene azaononga yonse ma boma nama ulamulilo na mpavu zonse. ²⁵ Chifukwa ayenela kulamulila mpaka aike bonse adani bake pansi pa mapazi yake. ²⁶ Mudani osilizila ni imfa. ²⁷ Chifukwa "anaika vonse pansi pa mendo yake." Koma pamene ikamba kuti "aika vonse," chionekelatu poyela kuti ichi sichi ikilapo pamozi nawamene anaika vonse pansi pake. ²⁸ Pamene vonse vi ikiwa pansi pa eve, pamene apo na Mwana mwamuna azaikiwa pansi pa uja wamene anaika vonse pansi pake, kuti Mulungu ankale onse mu bonse. ²⁹ Nanga kansi baja bamene bamabatiziwa kuimililako bokufa bazachita chani? Ngati bakufa sibaukisiwa, kansi nichani bamabatiziwa moimililako beve? ³⁰ Nanga nichani chamene tikungo nkala oyopesewa ntawi zonse? ³¹ Nifuka ola ili yonse ine! Ichi nichishininkisho monga mwamene ine nimazitukumulila pali imwe, kwamene nili nako mwa Kristu Yesu Mbuye watu. ³² Nanga pindu nichani, kuchiyanganila ku umuntu, ngati nina menyana na vinyama ku Efeso, ngati bakufa siba ukisiwa? "Lekani tidye na kumwa, chifukwa mailo tizamwalila." ³³ Musanamiziwe, "kunkala na bantu boipa ku-ononga nzelu zabwino." ³⁴ Nkalani ochenjela. Musapitilize kuchimwa. Pakuti benangu pakati kanu sibaziba Mulungu. Nikamba ichi kukuchitisani manyazi. ³⁵ Koma winangu azakamba kuti nanga bakufa baukisiwa bwanji ndipo bazankala nama thupi yabwanji? ³⁶ Ulibe nzelu iwe! Chintu chamene washanga sichizankala na moyo koma ngati chafa. ³⁷ Chamene ushanga situpi mwamene izankalila, koma ni mbeu chabe. Chizankala tiligu kapena chintu chinangu chabe. ³⁸ Koma Mulungu azacipasa tupi mwamene azafunila, ndiponso ku mbeu iliyonse tupi yake. ³⁹ Sima thupi yonse yolingana. Koma, kuli tupi ya banthu, ndipo ina ya vinyama, ndiponso inangu ya tunyoni, ndiponso ina ya nsomba. ⁴⁰ Kuli ma thupi yakumwamba ndiponso ya pa ziko yapansi. Koma ulemelelo wa thupi yakumwamba ni imozi na ulemelelo wa thupi yapaziko niyinu. ⁴¹ Pali ulemelelo wa zuba na ulemelelo wa mwezi, na ulemelelo wa nyenyezi. Pakuti nyenyezi imozi isiyana mu ulemelelo na nyenyezi inangu ⁴² Ndiye mwamene ku-ukisiwa kubakufa kulili. Chamene chishangiwa chimaonongeka, koma chamene chi-kusiwa sichi-onongeka. ⁴³ Chishangiwa chilibe ulemelelo; chi-ukisiwa mu ulemelelo. Chishangiwa chilibe mpavu; chi-ukisiwa na mpavu. ⁴⁴ Chishangiwa na thupi yachilengedwe; chi-ukisiwa na thupi ya uzimu. Ngati kuli thupi ya chilengedwe, kuli thupi ya uzimu. ⁴⁵ Monga mwamene chinalembelwa, "Muntu oyamba Adamu anankala na moyo." Adamu osiliza anankala muzimu-opasa moyo. ⁴⁶ Koma chaku uzimu sichinayambilile koma cha chilengedwe, kukonkapo chaku-uzimu ⁴⁷ Munthu oyamba niwapa ziko, opangiwa na doti. Muntu wachibili anachokela kumwamba. ⁴⁸ Monga mwamene eve anapangiwa ku doti alili, nimwamene balili baja banapangiwa ku doti, ndipo mwamene muntu wakumwamba alili, nimwamene balili baku ziko yaku mwamba. ⁴⁹ Monga

mwamene tinatengela chifanizo cha muntu waku doti, tiza tenga chifanizo cha muntu waku mwamba.⁵⁰ Manje ichi nikamba, abale, kuti thupi na mwazi sivinga tengeko mbali ya ufumu wa Mulungu. Chintu chamene chinga-onongeke sichinga landile chintu chamene sichi ma-onongeke.⁵¹ Onani! Lekani niku uzeni cha zo-ona chobisika: Sitizakafa bonse, koma bonse tizakachinjiwa.⁵² Tizakachinjiwa mwaka ntawi kangóno, mukupaila kwa linso, pakulila kwa lipenga yosilizila. Chifukwa lipenga izakalila, ndipo bokufa bazaka ukisiwa kunkala bosakwanilisiwa ku-onongeke, ndipo tizakachinjiwa.⁵³ Chifukwa iyi thupi yo-onongeke iyenela kuvala thupi yamene siyingaonongeke, ndipo iyi thupi ya imfa iyenela kuvala yosafa.⁵⁴ Koma pamene iyi thupi yo-onongeke yavala yosaonongeke napamene choonongeke chavala chosaonongeke ndiye pamene mau anena kuti,⁵⁵ "imfa kupambana kwako kuli kuti? Imfa, kuluma kwako kuli kuti?"⁵⁶ Ululu wa imfa ni chimo, na mpavu ya chimo ni lamulo.⁵⁷ Koma tiyamika Mulungu wamene atipasa kupambana kupitila mwa Ambuye Yesu Kristu.⁵⁸ Mwa ici, abale banga bokondewa, imililani molimba ndiponso mosa gwedesewa. Ntawi yonse kugwila ntchito ya Ambuye chifukwa muziba kuti ntchito yanu mwa Ambuye siyachabe.

Chapter 16

¹ Manje kukamba pali kusunkana kwa bantu ba Mulungu boyela: monga mwamene nina uzila mipingi za ku Galatiya, ndiye mwamene imwe muyenela kuchita nai mwe. ² Pa siku yoyamba sabata, ali onse pakati pa imwe afunika kusunga na kuika pambali monga mwamene akwanisila. Chitani ichi kuti kusakankale zo peleka pamene ine nizabwela. ³ Pamene ine nizabwela nizapeleka ma kalata yo zibisa bantu bamene imwe mu zindikila na kubatuma pamozi na mpaso yanu kupeleka ku Yerusalemu. ⁴ Ngati nichovomelesewa kuti na ine kuti niyende naine, baza endela pamozi na ine. ⁵ Koma nizabwela kuli imwe pamene nizapita mu Masedoniya. Chifukwa nizapita mu Masedoniya. ⁶ Penangu ninga nkale naimwe kwa ntawi itali kapena kunkala naimwe ntawi ya mpepo, kuti munganitandizile pa ulendo wanga, kwamene niyenda. ⁷ Chifukwa sinifuna kukuonani apa manje pamene nipita chabe. Niyembekezela kuti nika nkale na imwe ntawi yaitali kwambili, ngati Ambuye bavomelesa. ⁸ Koma nizankala mu Ifeso kufikila Pentekosti, ⁹ chifukwa chiseko chikulu chaseguka kuli ine, koma kuli badani bambili. ¹⁰ Manje pamene Timoti azabwela, onani kuti ali na imwe mosankala na manta, chifukwa achita ntchito ya Ambuye, monga mwamene ine nichitila. ¹¹ Mosavomelese muntu ali onse kuti amusule. Mutandizileni pamene ali munjila mumutedenle, mwakuti abwele kuli ine. Chifukwa nimuyembekezela kuti azabwela pamozi na ba bale. ¹² Manje pa za mubale watu Apolosi, ninamulimbikisa kwambili kuti aku endeleni imwe pamozi na babale. Koma sichinali chifunilo chake kuti akabwele manje. Koma, azakabwela pamene ntawi izankala yovomeleseka. ¹³ Nkalani bolangana, imililani molimbikila mu chikulupililo, nkalani monga bamuna, nkalani bolimba. ¹⁴ Lekani vonse vamene muchita vichitike muchikondi. ¹⁵ Muziba nyumba ya Stefanosi, kuti banali boyamba kunkala bokulupilila mu Akeya, na kuti bazipeleka ku ntchito ya bantu boyela ba Mulungu. Apa nikulimbikisani, babale, ¹⁶ kuti munkale bozipeleka kuli bantu ba mutundu uyu na kuli bonse bamene batandizila mu ntchito na kusebenzela pamozi na ise. ¹⁷ Nisekelela pa kubwela kwa Stefanosi, Fotyunetasi, na Akayakasi. Bakwanilisa kutandizila pamene imwe simulipo. ¹⁸ Chifukwa baukisa muzimu wanga na wanu. Mwa ichi, bazindikileni aba bantu ba mutungu uyu. ¹⁹ Mipingo za Eziya zipeleka moni. Akwila na Prisila baku pasani moni mwa Ambuye, pamozi na kachisi yamene ikumana mu nyumba mwabo. ²⁰ Bonse babale bakupasani moni. Pasani moni bonse na mpyompyono oyela. ²¹ Ine, Paulo, nilemba ivi na kwanja yanga. ²² Ngati muntu ali onse sakonda Ambuye, lekani ankale otembelelewa. Mbuye watu, bwelani! ²³ Chisomo cha Mbuye Yesu chinkale na imwe. Chikondi changa chinkale na imwe mwa Kristu Yesu. ²⁴ Koma ma lemba yambili yolemekezeka ya chi Giliki ya kudala maningi, na kuikilapo malemba yomasuliliwa yakudala, yalibe Amen posilizila malemba

2 Corinthians

Chapter 1

¹ Paulo, mutumiki wa Kristu Yesu kupitila mu chifunilo cha Mulungu, na Timoti mu bale watu, ku mpingo wamene uli ku Kolinto, na kuli bonse bantu ba Mulungu boyela mu malo yonse ya ku Akeya. ² Lekani chisomo chinkale naimwe na mutendele kuchokela kuli Mulungu Tate watu na Ambuye Yesu Kristu. ³ Lekani Mulungu na Tate wa Ambuye Yesu Kristu batamandiwe. Beve ndiye ba Tate ba chisomo komanso Mulungu wa kutontoza konse. ⁴ Mulungu amatitontoza mu ma vuto yonse, kuti naise tinga tontoze bonse baja bamene bali mu vovuta. Ise timatontoza benangu na kutontoza kumozu kwamene ise Mulungu anali kuti tontoza. ⁵ Monga mwamene kuvutika kwa Kristu kuma kula chifukwa chatu, chimozi-mozi kutontoza kwatu kuma kula kupitila mwa Kristu. ⁶ Koma ngati ise tivutika, nichifukwa cha kumvela bwino na kupulumusika kwanu; ngati ise timvesewa bwino, nikuti imwe mumvele bwino. Kumvela bwino kwanu kusebenza bwino mwa mpavu pamene imwe mupilila mukugabana mwa kuvutika kumozu-mozi kwamene ise timavutika. ⁷ Chiyembekezo chatu pali imwe sichi gwedezedka, chifukwa ise tiziba kuti pamene mutengako mbali mukuvutika, mutengako mbali mu kumvela bwino. ⁸ Sitifna kuti munkale bosaziba, abale, pali kuvutika kwamene tinankala nako mu Aziya. Tinali bogwedezeke kupitilila mwapu zatu mwakuti tina taya na chiyembekezo chosala na moyo. ⁹ Cha zo-ona, tinali nayo malemba a imfa muli ise. Koma ichi chinachitika kuti tisa ike chikulupililo chatu muli ise teka, koma muli Mulungu, wamene ama usha bakufa. ¹⁰ Eve anati pulumusa kuti chosa mu chiyembekezo choyofya, mu cha zoonazati pulumusa ise. Mwa eve ta ika chiyembekezo chatu kuti azatipulumusa. ¹¹ Azachita ichi pamene imwe mutandizila ise mu ma pempepo. Kukonkapo bambili bazapeleka ma yamiko kuimililako ise chifukwa cha mwai wamene unapelekewa kuli ise kupitila mu mapempepo ya bambili. ¹² Ise ndise bomvela bwino pali ichi: Mitima

zatu zipeleka umboni kuti ise tinazi sunga boyela na umulungu mu ziko, osati kuimilila pa nzelu za kutupi koma pa chisomo cha Mulungu. ¹³ Tilemba vintu osati vamene imwe simunga kwanise kubelenga kapena kumvela, ndipo chiyembekezo chatu nichakuti imwe muza mvesesa mofikapo ¹⁴ munga mwamene munamvesesa pangóno, mwakuti mungazitukumule pa siku ya Ambuye Yesu, munga mwamene ise timazitukumulila chifukwa cha imwe. ¹⁵ Chifukwa ninali na chisimikizo, ninali kufuna kubwela kuli imwe poyamba, kuti mulandile ma pindu ya kukutandalilani kabili. ¹⁶ Ninali kuganizila kuti nikuyendeleni pamene nizayenda ku Masedoniya. Nafuti ninali kufuna kukuyendelani pamene nizankala naulendo kuchoka ku Masedoniya, kuti imwe munilaile pamene niyenda ku Yudeya. ¹⁷ Pamene ine ninali kuganizila ichi, nanga ninali kukaika? Nanga nima konza vintu kukonka machitidwe ya bantu, kuti nikamba kuti "Inde, inde" kapena kuti "Iyayi, iyayi" pantawi imozi? ¹⁸ Koma munga mwamene Mulungu niokululupilika, sitikamba vonse kuti "Inde" na "Iyayi." ¹⁹ Chifukwa Mwana wa Mulungu, Yesu Kristu, wamene Siluvano, Timoti naine timamulalikila kuli imwe, sali kuti "Inde" nafuti kuti "Iyayi." Koma, eve ntawi zonse ali chabe kuti "Ind." ²⁰ Chifukwa ma lonjezo yonse mwa Mulungu mwa eve "Inde." Chimozi-mozi kupitila muli eve tikamba kuti "Inde" kupeleka ulemelelo kuli Mulungu. ²¹ Manje ni Mulungu wamene amasimikiza ise pamozi na imwe mwa Kristu, ndipo anatizosa, ²² anaika chidindo chake pali ise nakutipasa Muzimu mumitima zatu kunkala osimikizila ku vintu vamene vizabwela. ²³ Koma, ni itana Mulungu kuti ankale mboni wanga kuti chifukwa chamene sininabwelele ku Kolinto nichakuti ine niku siyeniko. ²⁴ Ichi sichifukwa chakuti tifuna kuti tiku lamulilani vintu vamene muyenela kukulupilila. Koma, ise tisebenzela pamozi naimwe kuti imwe munkale bokondwela, pamene muimilila muchikulupililo.

Chapter 2

¹ Chifukwa cha ichi ine ninaganizila kuti paine neka sinizabwelako futi uko mu vintu vovutisa. ² Ngati ninakulengesani vintu vobaba, nanga nindani wamene azanimvesa bwino koma imwe bamene muvutikisiwa chifukwa cha ine? ³ Ninalemba monga mwamene ninachitila chifukwa sinifuna ngati nabwela futi mukanimvese kuipa imwe bamene mufunika kunimvesa bwino. Nilinacho chikulupililo muli imwe kuti chimwemwe chamene ine nilinacho ndiye chamene naimwe muli nacho. ⁴ Chifukwa ine ninalemba movutikila kukulu, mopwanyika mutima, na misozi zambili. Sininafuni kuti nikulengeseni vobaba. Koma, Ninali kufuna kuti imwe muzibe kukula kwa chikondi changa chamene nilinacho pali imwe. ⁵ Ngati muntu ali one akulengesani vobaba, sanachite ichi chabe kuli ine, koma mwinangu-osati kuchikamba mwaukali-kuli imwe bonse. ⁶ Uku kulangiwa kwa muntu uyu na bambili kwakwana. ⁷ Manje makuti mumu lange, mukululukileni na kumu tontoza. Chitani ichi kuti asavutikisiwe kochila malile na vobaba. ⁸ Mwa ichi nikulimbikisani kuti pamenso pa bantu uyu muntu mulangiseni chikondi. ⁹ Ichi ndiye chifukwa chake chamene ninakulembelani imwe, kuti nikuyeseneni nakuziba ngati ndimwe bantu bomvelela mu vintu vonse. ¹⁰ Ngati imwe mukululukila muntu ali onse, naine uyo muntu namukululukila. Chintu chamene ine nakululuka-ngati nakululuka kantu kalikonse-ichi nachitila chifukwa cha imwe pamenso pa Kristu. ¹¹ Ichi chili mwa ichi kuti Satana asati name. Chifukwa tiziba ma ganizo yake. ¹² Ambuye bananisegulila chiseko pamene ine ninabwela ku m'zinda wa ku Tiloyas kuti nilalikile utenga wabwino wa Kristu kwame kuja. ¹³ Ninali ovutika ku muzimu chifukwa sinina mupeze mubale wanga Tayitas kwamene kuja. Ninabasiya naku yenda ku Masedoniya. ¹⁴ Koma mayamiko kuli Mulungu, wamene mwa Kristu ntawi zonse amatisogolela muku pambana. Kupitila muli ise ama peleka kununkila kwa bwino kwa nzelu za eve konse-konse. ¹⁵ Chifukwa ise kuli Mulungu ndise kununkila kwa bwino kwa Kristu, kuli bonse baja bamene bapulumuka nabaja bamene baonongeka. ¹⁶ Kuli baja bamene baonongeka, ndise kununkila kuchoka ku imfa kuyenda ku imfa. Kuli baja bamene bapulumusiwa, ndise kununkila kochokela ku umoyo kuyenda ku umoyo. Nanga nindani wamene ayenel aivi vintu? ¹⁷ Chifukwa ise sitili monga bantu bamene bagulisa utenga wa Mulungu kuti bapezepo ndalama. Koma, nama ganizilo yabwino, tikamba muli Yesu, monga mwamene titumiliwa kuchokela kuli Mulungu, pamenso pa Mulungu.

Chapter 3

¹ Nanga tiyamba kuzi tamanda paise teka futi? Ise sitifunika ma kalata yoti tokoza yochokela kuli imwe kapena yopasa imwe iyayi, monga bantu bena, nanga tifunika? ² Imwe paimwe mweka ndimwe ma kalata yatu yokamba zabwino pali ise, yolembewa pa mitima zatu, yozibika nafuti yobelengeka na bantu bonse. ³ Muma onesa kuti ndimwe kalata yochokela kuli Kristu, yopelekewa na ise. Iyi si inalembewe na cholembela koma yolembewa na Muzimu wa Mulungu wa moyo. Siyana lembewe pa tolembelapo topangiwa na malibwe iyayi, koma cholembelapo chamene ni mitima za bantu. ⁴ Ichi ndiye chi kulupililo chamene ise tilinacho mwa Kristu pamenso pa Mulungu. ⁵ Ise sindise boyenela kuti tikambe kantu kali konse kuti kachokela kuli ise. Koma, kukwanilisa kwatu kuchokela kuli Mulungu. ⁶ Ni Mulungu wamene anati lenga kunkala batumiki bokwanila ba pangano ya manje. Iyi pangano siyamene yo chita kulemba kalata koma ya Muzimu. Chifukwa malemba yama paya, koma Muzimu upasa moyo. ⁷ Manje utumiki wamene unalenga imfa-wamene una dindiwa mumalemba pa mabwe-unabwela mu ulemelelo ukulu wakuti bana ba Islayeli sibanali kukwanisa kumulanga pamenso Mose. Ichi chinali chifukwa chakuti pamenso pake panali ulemelelo, ulemelelo wamene unali kusila. ⁸ Nanga kuchilapo kwa kusebenza kwa Muzimu kansi ndishi kuzankala kwa bwanji? ⁹ Chifukwa ngati utumiki wa chionongeko unali na ulemelelo, onani kuchilapo kwa kusebenza kwa chilungamo mwamene kuchililapo mu ulemelelo! ¹⁰ Chifukwa mu cha zoona, chija chamene chinali chinalengewa kunkala na ulemelelo chinkala chilibe na ulemelelo mukuganiza uku, chifukwa cha ulemelelo wamene uuchila. ¹¹ Chifukwa ngati chintu chamene chinali kupita chinali nao ulemelelo, kansi nanga ulemelelo wa chintu chamene sichisila uzankala wa bwanji! ¹² Kansi pakuona kuti tili nacho chiyembekezo cha mutundu uyu, ndiye bozilimbisa. ¹³ Ise sitili monga Mose, wamene anaika chitambala chomubisa pa menso kulengesa kuti bana ba Islayeli basakwanise kulangana mwamene kunali kusila kwa ulemelelo wamene unali kuyenda kusila. ¹⁴ Koma nzelu zao zinali zobisika. Chifukwa kufikila lelo, pamene beve babelenga pangano yakudala, chija chitambala chobisa pamenso chikalipo. Sichina chosewepo, chifukwa ni muli Kristu mweka mwamene chimachosewapo. ¹⁵ Kunkala nalelo, pamene Mose abelengewa, chinyula chikali kubisa mitima zao. ¹⁶ Koma ngati muntu atembenukila kuli Ambuye, ichi chinyula chima chosewapo. ¹⁷ Manje Ambuye ndiye Muzimu uyu. Kwamene kupezeka Muzimu wa Ambuye, kuli kunkala omasuka. ¹⁸ Manje ise tonse, na pamenso posa bisika, ti u-ona ulemelelo wa Ambuye. Tichinjiwa kuti tinkale chimozi-mozi maonekedwe kuchokela ku ulemelelo wa pamalo yamozi kuyenda pa ulemelelo wapamwamba, monga kuli Ambuye, wamene ndiye Muzimu.

Chapter 4

¹ Chifukwa cha ichi, pakuona kuti tili nao utumiki uyu, nakuona kuti tinalandila chisomo, sitinkala wobwezewa kumbuyo. ² Koma, tinakana njila zobisika koma futi zansoni. Ise sitinkala na nzelu zochenjelesa, nafuti ise siti sebenzesa mau ya Mulungu munjila yosayenela. Pa kupeleka vazo-ona, timazi tamanda pateka mu mitima za bantu bonse pa menso pa Mulungu. ³ Koma ngati utenga watu ubisika, ubisika chabe kuli baja bamene baonongeka. ⁴ Kwa beve, mulungu wa ino ziko ana bisa nzelu zabo zosa kululupila. Pindu yake niyakuti, sibakwanisa kuona ku unika kwa utenga wa ulemelelo wa Kristu, wamene ndiye chitunzi-ntunzi cha Mulungu. ⁵ Chifukwa ise sitizilalika, koma Kristu Yesu monga Mbuye, na ise monga bakapolo banu Kuchitila Yesu. ⁶ Chifukwa Mulungu niwamene anakamba kuti, "Nyali izaonekela kuchokela mu mu finzi." Eve aonesela ku unika mu mitima zatu, kuti apeleke ku unika kwa nzelu za ulemelelo kwa Mulungu pamenso pa Yesu Kristu. ⁷ Koma tili na chuma ichi mu mbiya za doti, mwakuti chinkale po onekelatu kuti kuchilapo kwa ukulu wa mpavu nikwa Mulungu osati chifukwa cha ise iyayi. ⁸ Ise tima vutikisiwa konse-konse, koma si tima gwesewa. Timadabwisiwa koma sitima taya chikulupililo. ⁹ Timasausiwa koma sitima lekelewa; kuchaiwa koma osati kuonongeka; ¹⁰ ntawi zonse kungonyamula muma tupi yatu imfa ya Ambuye Yesu, kuti umoyo wa Yesu ungaoneseleke muma tupi yatu. ¹¹ Chifukwa ise bamene tili na moyo timapelekewa ku imfa chifukwa cha Yesu, kuti umuyo wa Yesu uonekele mu ma tupi yatu ya yamene ya mafa. ¹² Mwa ichi imfa isebeza muli ise, koma umoyo usebeza mukati mwanu imwe. ¹³ Koma tili naye muzimu umozi wa chikulupililo kulingana na chamene china lembewa: "Ninakulupilila, nakukamba." Naise tikulupilila, kulingana kwamene tikamba, ¹⁴ chifukwa tiziba kuti wamene ana ukisa Ambuye Yesu azati usha naise pamozi na Yesu nakuti leta ise pamozi na imwe pamaso pake. ¹⁵ Chifukwa vonse ni kuchitila imwe imwe, mwakuti chisomo chamene chifikila bantu bambili-mbili chingalenge bantu kupeleka mayamiko yambili ku ulemelelo wa Mulungu. ¹⁶ Chifukwa chake ise sitibwezewa kumbuyo. Ngakale kuti kunja tiyenda tisila, koma mukati tiwamiziwa siku na siku. ¹⁷ Pakuti ichi chintu cha ntawi ingono, kuvutika kwa pan'gono kuti konzesela kuti tikalandile ulemelelo wosasila wamene upitilila mapimidiwe yonse. ¹⁸ Chifukwa ise sitilanga chabe kuyembekezela vintu vamene vioneka iyayi, koma vintu vamene sivioneka. Vintu vamene vioneka niva kantawi kangono chabe, koma vintu vamene sivioneka niva ntawi yosasila.

Chapter 5

¹ Tikiba kuti ngati iyi nyumba yonkalamo yapa ziko ikaonongekewa, tilinayo yomangiwa na Mulungu. Iyi si nyumba yomangiwa na manja ya bantu, koma nyumba yamuyayaya, kumwamba. ² Chifukwa muli iyi nyumba ti buluwa, kufunisisa kuti tivalikiwe na nyumba yatu ya kumwamba. ³ Tifunisisa ichi chifukwa chakuti tiyaivala sitizapezeka bosavala. ⁴ Chifukwa pamene tili muli iyi nyumba, tibuluwa, onkala bolemesewa. Sitifuna kuti tinkale bosavala. Koma, tifuna kuvalikiwa, kuti chamene chili cha imfa chi melewe na moyo. ⁵ Eve wamene anatikonzela ivi vintu ni Mulungu, wamene anatipasa Muzimu kunkala oshininkishila wa vintu vamene vizabwela. ⁶ Mwa ichi nkalani ntawi zonse bolimba mutima. Nkalani bochenjela kuti pamene tili pa nyumba mu tupi, sitili kuli Ambuye. ⁷ Chifukwa tiyenda mu chikulupililo, osati kukonka vamene tiona. ⁸ Chifukwa chake ndise bolimba mutima. Tingasankepo kunkala kutali na tupi kuti tinkale na Ambuye. ⁹ Chifukwa chake tichipanga kunkala lingo yatu, kuti ngakale tili pa nyumba kapena kutali, kumumvesa bwino. ¹⁰ Chifukwa tiyenela kuonekela kuweluziwa pa mupando wa Kristu, kuti ali onse alandile vabo kulingana na vintu vamene bana chita mutupi, vabwino kapena voipa. ¹¹ Mwa ichi, mwamene tizibila chiopezo cha Ambuye, tipapatila bantu. Mwamene tilili timaonekela kuli Mulungu, nikulupilila kuti chili poonekela na mumitima zanu. ¹² Sitiyesa kuku patikizani kuti muti one monga ndise bantu bachilungamo, koma, tikupasani chifukwa chakuti munkale bomvela bwino pali ise, kuti mungankale nayo yanko kuli baja bamene bamazitukumula pa maonekedwe osati pa vamene vili mumutima. ¹³ Chifukwa ngati ndise bosokonezeka, tichitila Mulungu; koma ngati ndise bokwanila chabe bwino bwino, tichitila imwe. ¹⁴ Chifukwa chikondi cha Kristu chitikakamiza, chifukwa tizibisisa kuti: Kuti muntu umozi anafela bantu bonse, nakuti bonse bana mwalila. ¹⁵ Anafela bonse, kuti baja bamene bankala na moyo basazinkala myoyo zabo beka chabe koma kunkalila Eve wamene kamba ka beve anabafela koma futi anaukisiwa. ¹⁶ Chifukwa cha ichi, kuyambila apa sitiweluziwa muntu kulingana na mankazikidwe ya umuntu, ngakale kuti pa ntawi ina tinamuganizila Kristu munjila iyi. Koma manje siti ona muntu ali onse munjila iyi nafuti. ¹⁷ Mwa ichi, ngati muntu ali onse mwa Kristu, eve niwopangiwa manje. Vintu vakudala vapita. Onani, vankala va manje. ¹⁸ Ivi vintu vonse vichokela kuli Mulungu. Anati bweza kuli eve kupitila muli Kristu nakutipasa utumiki wobwezesana ubwenzi. ¹⁹ Kutantauza kuti, muli Kristu Mulungu abweza ziko kuli eve, osati kuipendela ma chimo ziko. Eve akululupilisa utenga wa kubwezana kuli ise. ²⁰ Chifukwa chake ise tinkazikiwa kunkala boimililako Kristu, kuchita monga Mulungu apapatila kupitila muli ise. Tikupapatani, chifukwa cha Kristu: "Bwelelani kuli Mulungu!" ²¹ Analenga Kristu kunkala nsembe ya machimo yatu. Eve niwamene sanachimwepo. Anachita ichi kuti ise tinkale chilungamo cha Mulungu muli eve.

Chapter 6

¹ Kusebenzela pamozi na eve, tikulimbikisani kuti musalandile chisomo cha Mulungu mwa chabe. ² Chifukwa akamba, "muntawi yovomelesewa ninakuikanikoni nzelu, na pantawi ya chipulumuso ninakutandizani." Onani, apa manje ndiye ntawi yovomelesewa. Onani, manje apa ndiwe ntawi ya chipulumuso. ³ Ise siti ikapo chokugwesani pa pasogolo kwanu, chifukwa sitifuna utumiki watu kuti unyozewe. ⁴ Koma, tizionesela kupitila muma chitidwe yatu, kuti ise ndise bakapolo ba Mulungu. Ndise bakapolo bake mu kulimbikila, vovuta, manta, volimba, ⁵ kumenyewa, mu ndende, musokonezo, mukusebenza kwa mpavu, usiku oakangiwa kugona, ntawi ya njala, ⁶ kunkala oyela, nzelu, kulindilila, kunkala wabwino mutima, mumu Zimu Oyela, mu chikondi cha zo-ona. ⁷ Ise ndise bakapolo bake mu mau ya cha zo-ona, mu mpavu za Mulungu. Vovala va chilungamo vaku kwanja la kwanja na kwanja yaku manzele. ⁸ Timasebenza pa ulemu napamene palibe ulemu, monyozewa na pa matamando. Ise tinamiziliwa kuti ndise ba boza koma ndise bachilungamo. ⁹ Tisebenza monga sitizibika koma tizibika bweino. Tisebenza monga tikufa koma-onani!-tikali nao umoyo. ¹⁰ Tisebenza monga bolila, koma tinkala bosangalala ntawi yonse. Tisebenza monga bosauka, koma tilenga bambili kulemela. Tisebenza monga baja bamene balibe kalikonse koma tili navo vintu vonse. ¹¹ Takamba vonse va zooni kuli imwe, Akolinto, na mutima watu nioseguka. ¹² Imwe simulesewa na ise, koma mulesewa mweka mu mitima zanu. ¹³ Manje kuti ninkale okuganizilani-nikamba monga nikamba na bana-naimwe langizani mitima zanu zonse. ¹⁴ Musankale pamozi nabaja bosakulupilila. Nanga ni chi bwenzi chabwanji chamene chilungamo chimankala nacho na bosakonka malamulo? Nanga ni ubwenzi uti wamene nyali imankala nacho na mfinzi? ¹⁵ Nanga nikumvelana kwa bwanji kwamene Kristu ali nako na Belaya? Kapena nimbali bwanji yamene eve okulupilila ali nayo na uja osakulupilila? ¹⁶ Kapena niku mvelana kwa bwanji kwamene kuli pakati pa nyumba ya Mulungu naya tu milungu topanga? Chifukwa ise ndise nyumba ya Mulungu wa moyo, monga mwamene Mulungu anakambila kuti: "Nizankala pakati pabo naku enda pakati pabo. Nizankala Mulungu wabo, na beve bazankala bantu banga." ¹⁷ Mwa ichi, "Chokani koni kuli beve, nkalani bopatuliwa," bakamba Ambuye. "Mosagwila chintu chamene chili na doti, ndipo ine nizakulandilani. ¹⁸ Nizankala Tate kuli iwe, naimwe muzankala bana banga bamuna naba kazi,"mwamene bakambila Ambuye Bampavu.

Chapter 7

¹ Bokondewa, pakuona kuti tili nayo ma lonjezo aya, lekani tizisuke kuchosa vintu vonse vamene vitilenga kunkala badoti mu tupi na mumuzimu. Lekani tikonkelese kunkala boyela moyopa Mulungu. ² Tikonzeleni ponkala mumitima zanu ise! Sitina lakwile muntu ali onse. Sitina ipise muntu ali onse kapena kusebenzesa muntu kwa chabe. ³ Sinikamba ichi kuti nikupezeni na choipa iyayi. Chifukwa nakamba kudala kuti imwe muli mu mitima zatu, kuti ise tikafele pamozi na kunkala pamozi. ⁴ Nilinacho chikulupililo muli imwe, ndipo nima mvela bwino chifukwa cha imwe. Ndine ozula na kumvela bwino. Nitaikila na kukondwela ngakale nili na vovuta vamene nipitamo. ⁵ Pamene ise tina bwela ku Masedoniya, ma tupi yatu siyanapumule. Koma, tinali wovutika munjila ili yonse na mavuto ya kunja na manta mukati mwatu. ⁶ Koma Mulungu, wamene ama tontoza baja bobwezewa kumbuyo, anati tontoza na kubwela kwa Taitas. ⁷ Sikunali chabe kubwela kwake kwamene Mulungu anati tontoza iyayi. Koma na tontozo yamene Taitas analandila kuli imwe. Anati uza pa va kuvutika kwanu, chisoni, na kutiganizila kwanu kwapatali. Chifukwa chakwe ine ninakondwela maningi futi. ⁸ Ngakale kuti kalata yanga inaku mvesani kuipa, sinimvela kuipa pali vamene nina lemba iyayi. Koma ninamvela kuipa pamene ninaona kuti kalata yanga inaku lengani kunkala wopwanyika mutima, ngakale kuti ichi chinali cha kantawi kang'ono chabe. ⁹ Koma apa manje ine nisekelela, osati chifukwa imwe muna mvela kuipa, koma chifukwa chakuti kumvela kuipa kwanu kunalenga kuti mutembenuke. Munamvela kuipa kwa umulungu, chifukwa chake imwe simuna tayepo kali konse chifukwa cha ise. ¹⁰ Chifukwa chakuti kumvela kuipa kwa umulungu kumalengesa chipulumuso chamene simunga mvele kuipa nacho. Kumvela kuipa kwa pa ziko, kweve, kumaleta imfa. ¹¹ Onani kuwama mukati mwanu mwamene kufunisisa maningi kwalengesewa na kumvela kuipa. Onani ukulu wofunisisa wa mukati mwanu kufuna kuonesasa kuti sindimwe bolakwa. Ukulu wa ukali wanu, manta yanu, kufunisisa kwanu, mwafunisisa kuti muone kuti chilungamo chichitike, na kufunisisa maningi kwanu kuti chilungamo chichitike! Mu vonse mwaonesa kuti imwe mulibe kolakwa mu chintu ichi. ¹² Ngakale kuti ninalemba kuli imwe, sininalembele chabe chifukwa cha uja olakwa, kapena uja wamene analakwiliwa, koma mwakuti ubwino wanu kuli ise uwonekele kuli imwe pa menso pa Mulungu. ¹³ Ichi ndiye chifukwa chake ise tilimbisiwa. Kuikilapo pa tontozo yatu, tinasekelelela maningi chifukwa cha chimwemwe cha Tito, chifukwa muzimu wake unali omvela bwino chifukwa cha imwe monse. ¹⁴ Chifukwa ngati ine ninamvela bwino pali imwe, sinina mvele nsoni. Koma, monga mwamene vonse tinakamba kuli imwe vinali va zoona, kumvela bwino kwatu pali imwe kuli Taitas kunaonesewa kuti nikwazoona. ¹⁵ Chikondi kwake pali imwe ni chikulu pamene akumbukila kumvela kwanu, mwamene muna mu landilila mwa manta na kunjenja. ¹⁶ Nisekelela chifukwa nili na chikulupililo muli imwe.

Chapter 8

¹ Tifuna imwe muzibe, abale, pa chisomo cha Mulungu chamene china pasiwa kuli mipingo zaku ma kachisi yaku Masedoniya. ² Mukati mwa vovuta, kukula kwa kusekelela kwabo na kusauka kwabo valengesa kupaka kwa kulemela kwa mu zopasa. ³ Chifukwa nipeleka umboni kuti banapeleka kwambili monga mwamene wanali kukwanilisa, na kupitilila malile yabo, na mopeleka chabe mofuna mwabo ⁴ banatipapatila kuti batengeko mbali kusankiwa kuti mukupeleka zopeleka mu utumiki wa Mulungu kuli boyela bapelekeko na beve. ⁵ Koma ichi sichina chitike monga mwamene ise tinali kuganizila, koma banayamba kuzipele poyamba kuli Ambuye kukonkapo nakupeleka kuli ise monga muchifunilo cha Mulungu. ⁶ Tinalimbikisa Taitas, wamene anyamba kudala iyi ntchito, kuti aisilize pakati kanu iyi ntchito ya chisomo. ⁷ Koma imwe kulani mu vonse-mu chikulupilo, kakambidwe, nzelu, muku onesesa, na muchikondi chanu kuli ise. Mwa ichi onesesani kuti mu chilapo muli machitidwe aya ya chisomo. ⁸ Koma nikamba ichi osati monga lamulo. Koma, nikamba ichi kuti niyese kuti chikondi chanu nichazo-ona paku chilinganiza na kufunisisa kwa bantu benangu. ⁹ Chifukwa imwe muziba chisomo cha Ambuye Yesu Kristu. Ngakale kuti banali bolemela, chifukwa cha imwe banankala bosauka, kuti kupitila muli kusauka kwabo imwe munga lemele. ¹⁰ Pali ichi cheve nizaku pasani nzelu zamene zizakutandizani. Chaka chimozi kumbuyo uku, simu nayambe chabe kuchita chintu, koma munali kufuna kuchichita. ¹¹ Manje chitani. Monga mwamene munalili ofunisisa maningi kuchita paga, onesesani kuti mukwanilise kusilizisa, kulingana na mwamene mungakwanilisile. ¹² Chifukwa ngati imwe mufunisisa kuchita chintu ichi, nichintu chabwino koma futi chovomelesewa. Chiyenela kulingana na mwamene muntu alinacho, osati monga chintu chamene alibe. ¹³ Koma iyi ntchito siyakuti imwe mulemesewe na vambili benangu balekelelewe iyayi. Koma, kufunika kunkala kulinganisa. ¹⁴ Kuchulukila kwanu pa ntawi iyi izatandizila vamene bafuna. Ichi futi nichakuti kulemela kwabo kungatandizile vofunikila vanu, nafuti kuti kunkale kulinganiza. ¹⁵ Chili monga mwamene vilili: "Uja anali na vambili kulibe kamene anasala nako, nauja wamene anali na tungono sana pelebe kali konse." ¹⁶ Koma matamando kuli Mulungu, wamene anaika mu mutima wa Taitas kusamalila kwazo-ona kwamene monga ine nili nako. ¹⁷ Sana vomele chabe kupempa kwatu chabe, koma anali wokululukilika pali ivi. Anabwela kuli imwe mozifunila eve eka. ¹⁸ Tamutumizila pamozi na mubale watu wamene amatamandiwa mu mipingo yonse chifukwa cha kasebenzedwe kake mu kulalika utenga wabwino. ¹⁹ Osati ichi chabe iyayi, koma anasankiwa futi na mipingo kuti ayendele pamozi naise mukugwila ntchito iyi ya chisomo. Ichi chili njila kuti tipeleke ulemu kuli AMbuye beka na kufunisisa kwatu kuti titandize. ²⁰ Ise sitifuna kuti muntu ali onse ankale nadandaulo pali ise chifukwa cha kupasa kwamene ise tipasa. ²¹ Tionesesa kuti tichite chintu chamene chili naulemu, osati pa menso pa Ambuye peka, koma na pamenso pa bantu. ²² Tizatuma futi mubale winangu pamozi nabeve. Ise tinamu yesa munjila zosiyanasiyana koma tinamu peza okululupilika muzi ntchito zambili. Niofunisisa manje chifukwa cha chikulupililo chamene ali nacho muli imwe. ²³ Pali Taitas, eve niosebenzela pamozi naine nafuti osebenzela pamozi naye kuli imwe. Pali babale batu, banatumiwa na mipingo. Nibopeleka ulemu kuli Kristu. ²⁴ Mwa ichi balangizeni chikondi, nafuti langizani ku mipingo kumvela bwino kwamene ise timakambo pali imwe.

Chapter 9

¹ Kulingana pali ntchito yosebenzela bantu ba Mulungu boyela, sichoyenela kuti ine nikulembeleni kalata imwe. ² Niziba kufunisisa kwanu, kwamene ine nimazitukumulilapo kuli bantu baku Masedoniya. Ninabauza kuti Akeya inayamba kukonzekela kuyambila chaka chasila. Kufunisisa kwanu kwalengesa kuti bantu bambili basebenze. ³ Manje ine natuma babale kuti kuzitukumula kwatu pali imwe kusankale kwachabe, na kuti imwe munkale bokonzekela, monga mwamene ninakambila kuti munkalile. ⁴ Ndaba, ngati bantu baku Masedoniya bakabwela pamozi na ine naku peza kuti imw simunakonzekela, ise tizamvela nsoni-sinikamba choipa pali imwe iyayi-koma chifukwa chonkala okukulupililani imwe. ⁵ Mwaichi naganizila kuti chinali choyenela kuti nilimbikise babale kuti babwele kuli imwe naku konza mpaso yanu mwamusanga yamene imwe muna lonjeza. Ichi ndiye kuti inkale yokonzekelatu monga daliso, osati monga chintu choku kakamiza. ⁶ Chamene tikamba ni ichi: Wamene ashanga nakaso azakolola tungóno, na uja wamene ashanga kuti alandile daliso azalandila daliso. ⁷ Lekani muntu ali onse apeleke monga mwamene aganizila mumutima wake, osati mokaikila kapena mokakamiza, chifukwa Mulungu akonda uja muntu opeleka mosangalala. ⁸ Mulungu akwanisa kulenga kuti chisomo chonse chilefukile imwe, kuti, mu vintu vonse, mungankale na vonse vintu vamene mufuna. Ichi chizankala njila iyi kuti mungalengese kuchuluka kwa ntchito ili yonse. ⁹ Chili monga mwamene chinalembelewa: "Agabisa chuma chake nakupasa baja bosauka. Chilungamo chake nicha muyayaya." ¹⁰ Eve wamene amapeleka mbeu kuli mulimi wamene amashanga na mukate kuti badye aza peleka na kukulisa mbeu yanu chifukwa chakuti mwa shanga. Eve azakulisa kukolola kwa chilungamo. ¹¹ Muzalemela mu njila ili yonse kuti mungankale bamutima bopasa. Ichi chizalengesa kuti maymiko yaende kuli Mulungu kupitila muli ise. ¹² Pakugwila ntchito iyi sikuma kwanisa chabe ku tandizila vofunikila va bantu boyela ba Mulungu, koma chimalefukila munjila zosiyanasiyana zotamanda Mulungu. ¹³ Chifukwa cha kuyesa kwanu na kusimikisiziwa kwanu mu ntchito iyi, imwe muzapeleka ulemelelo kuli Mulungu kupitila muli mutima opeleka wa mpaso kuli beve na kuli bonse. ¹⁴ Beve bafunisisa imwe, koma nafuti bakupempelelani imwe. Bachita ichi chifukwa cha ukulu wa chisomo cha Mulungu chamene chili pali imwe. ¹⁵ Mayamiko yankale kuli Mulungu chifukwa cha mpaso yake yamene mau siyangakwanise kuikamba!

Chapter 10

¹ Ine, Paul, paneka nikupempani imwe, kupitila mu kuzichepesa na ulele wa Kristu. Ndine ozichepesa ngati nili naimwe. koma ndine olimba mutima kuli imwe ngati nili kutali na imwe. ² Nikupempani kuti, pamene nizankala naimwe, sinizankala olimba mutima na kuzimvela. Koma niganizila kuti nizafunikila kunkala olimba mutima pamene nishushana baja bamene bashusha kuganiza kuti ise tinkala monga kulingana na zaku tupi. ³ Ngakale kuti ise tiyenda nama tupi, sitima menya nkondo monga bantu. ⁴ Chifukwa vankondo watu vamene timenyela siva kutupi. Koma, vili nayo mpavu ya umulungu kuononga maganizo. Yamalengesa kuti kunkale kuli pindu kuli bohusha. ⁵ Tiononga futi vonse vintu vamene vizikwezeka kushusha nzelu za Mulungu. Timatenga maganizo yonse ukapolo kuti yamvele Kristu. ⁶ Ndipo tinkala bokonzekela kuti tilange chintu chili chonse chosakonka lamulo, pamene naimwe kumvela kwanu kukwanisika. ⁷ Langanani pali chintu chamene chili pasogolo panu. Ngati muntu ali onse akulupilila kuti eve niwa Kristu, lekani kuti azikumbuse eve eka kuti mwamene eve ali wa Kristu, naise nimwamene tilili. ⁸ Ngakale kuti ine nizimvela pang'ono pali mpavu zatu, zamene Ambuye banatipasa kuti tikulise imwe osati kuti tiku onongeni imwe, sinizamvela nsoni iyayi. ⁹ SInifuna kuti chioneke monga ine nikuyofyani nama kalata yanga aya. ¹⁰ Chifukwa bantu benangu bakamba kuti, "ma kalata yake yalibe masobela ndipo niyakali, koma maonekedwe aoneka alibe mpavu. Mau yake siyaja yotailako nzelu." ¹¹ Bantu aba balekeni bankale boziba kuti mwamene ise tilili mu ma kalata pamene sititonse naimwe ndiye mwamene ise tizankalila mumachitidwe pamene tizankala pamozi naimwe. ¹² Ise sitienda kutali kochita kufika kuzi ika mutuma gulu gulu kapena kuzilinganisana nabaja bamene bamazitamanda beka. Koma beve bakazipima pabeka beka wina na muzake nakuzilinganisana beka, balibe nzelu. ¹³ Ise, koma, sitinga zitukumule kupitilila malile. Koma, tizachita ichi molinganila chabe kulingana na mwamene Mulungu ativomelesela ise, kulinganisa nakwamene kufikila kuli imwe. ¹⁴ Chifukwa ise sitinazilengese kuti tizifikise kuli imwe. Tinali boyamba kufikila konse uko kuli imwe na utenga wa Kristu. ¹⁵ Ise sitina zitukumule kuchila malile pali ntchito ya benangu. Koma, chiyembekezo chatu nichakuti chikulupililo chanu chipitilize kukula, ntchito yatu pakati panu izakula maningi. ¹⁶ Tiyembekeza maningi ichi, kuti tingalalikile utenga kuikilako malo yamene yali kumalo yopitilila kwanu uko. Ise sitizitukumula pa ntchito yamene ichitiwa mumalo ya winangu ¹⁷ "Koma lekani eve wamene azitukumula, azitukumule mwa Ambuye." ¹⁸ Chifukwa siuja wamene akamba zabwino pali eve eka wamene avomelesewa. Koma, niuja wamene Ambuye bavomelesa.

Chapter 11

¹ Ningafune kuti mungani vomelese muvinangu vilibe nzelu. Koma zo-ona muni vomeleza ine! Ine nili na kaduka pali imwe. ² Nili na kaduka ka umulungu pali imwe, chifukwa ine nina lonjeza imwe ukwati kuli mwamuna umozi. Ninalonjeza kuti nizakupelekani moye oyela kuli Kristu. ³ Koma nili manta chifukwa chakuti mwinamwake, monga mwamene chija chinjoka chinanamila Eva nakuchenjela kwake, maganizo yanu yangataiwe kuchosewa kuzipeleka kwa zo-ona kuli Kristu. ⁴ Chifukwa ganizani kuti wina abwela na kulalika Yesu wina osati wamene tinalalikila. Kapena ganizani kuti mwalandila muzimu osiyana na wamene munalandila. Kapena ganizani kuti mwalandila utenga wina osiyana na wamene munalandila. Imwe munapilila na ivi vintu mofikapo. ⁵ Chifukwa ine niganiza kuti sindine osalila kuli baja bamene bamaitaniwa kuti kuti niba tumiki bapamwamba. ⁶ Koma ngakale kuti ine sindine opunzisiwa mokambila, koma sindine uja osapunzisiwa mu nzelu. Munjila ili yonse na mu vintu vonse tinakuzibisani ivi vintu. ⁷ Nanga ninachimwa kansi pa kuzichepesa kuti imwe mukezekewe? Chifukwa ine ninalalikila utenga wabwino wa Mulungu kuli imwe mosalipilisa. ⁸ Ninabela ma mipingo zinangu mu kuvomela kutandiziwa na beve kuti ine nisebenzele imwe. ⁹ Pamene ninali na imwe nafuti pame nenze kufuna kantu, sininavute muntu ali onse. Chifukwa vofuna vanga vinatandiziwa na babale banga bamene bana bwela kuchokela ku Masedoniya. Mu vintu vonse ine ninazi lesa kuti ninkale cholemesa kuli imwe, nafuti ine nizapitiliza kuchita chamene ichi. ¹⁰ Monga mwamene cha zo-ona cha Krsitu chili muli ine, uku kuzitukumula kwanga sikuzalesewa mu ma del yaku Akeya. ¹¹ Chifukwa? Chifukwa ine sini kukondani? Mulungu aziba. ¹² Futi chamene nichita nizapitiliza kuchichita, kuti ninga tenge mpavu ya baja bamene bamani peza olakwa nakukamba kwabo kwamene bazitukumulila-kuti bapezeka bachita ntchito imozi yamene ise tichita. ¹³ Chifukwa aba bantu ni batumiki baboza nafuti bantchito baboza. Bamazi bisa kuzionesa monga nibatumiki ba Kristu. ¹⁴ Futi ichi chintu sichodabwisa, chifukwa na eve Satana amazionesa monga ni mungelo wa ku unika. ¹⁵ Si chintu chodabwisa kuti naba ntchito bake bamazilangiza monga bantchito bachilungamo. Chosilizila chabo chizankala monga vochita vabo. ¹⁶ Nikamba nafuti kuti: Osaleka muntu ali onse aniganizile kuti ine ndine chipuba. Koma ngati muganiza ivi, nilandileni monga ndine hcipuba kuti ninga zitukumuleko pangóno. ¹⁷ Chamene nikamba mukuzitukumula kozivensa-Sinikamba monga mwamene Ambuye bangachitile-Koma nikamba monga chipuba. ¹⁸ Chifukwa bantu bambili bamazitukumula kulingana na vakutupi, naine nizazitukumula. ¹⁹ Imwe munalekelela vipuba na chimwemwe. Imwe ndimwe banzeli! ²⁰ Chifukwa imwe munamukwanisa wamene amaku lengani kunkala bakapolo, ngati akudyani imwe, ngati azi pindullila pali imwe, ngati aziona kuti niopitilila pali imwe, kapena ngati akumenyani mbama pa menso. ²¹ Nizakamba ichi cha nsoni kuli ise kuti ise tinalibe mpavu kuti tichite ichi. Koma ngati ali onse azitukumula-Nikamba monga chipuba-naine nizazitukumula. ²² Nanga niba Heberi? Naine nimwamene nilili. Nanga niba Islayeli? Naine ndine mu Islayeli. ²³ Nanga niba tumiki ba Kristu? (Nikamba monga nzelu zanga sozikwana.) Ine nichilapo apa peve. Ninankala mu ntchito yochilapo kulimba, mu ndende kambili kuchilapo, ku menyewa kopitilila malile, mukukumana voyopesa vambili va imfa. ²⁴ Kuli ba Yuda ninalandila mikwapu "makumi yanai kusiyapo kamozi." ²⁵ Katatu ninamenyewa na ndodo. Kamozi ninatemewa myala. Katatu chibwato chinatipwanyikila pa manzi. Ninkala pa mumana zuba na usiku umozi. ²⁶ Ninankala pamaulendo yambili pafupi pafupi, kuyopesewa pa mimana, mu kuyopa vigabenga, kuyopa bantu banga, kuyopa bakunja, kuyopa mu muzinda, kuyopa mu chipululu, mukuyopa mu nyanja, mukuyopa babale baboza. ²⁷ Ninankala pa ntchito yolimba na mu mavuto, usiku unalibe tulo, mu njala na njota, kambili kusadya chakudya, mu mpepo na mu maliseche. ²⁸ Kuchoselako ivi vonse, kuli maganizo yosamalila mipingo yamene nima nkala nayo. ²⁹ Nanga nindani wamene eali ofoka, ine nankala osafokelamo naine? Nindani wamene analengesewa kugwa, naine sinina pyele kumozi? ³⁰ Ngati ine ningazitukumule paneka, nizazitukumula pali vamene vilangisa kusankala na mpavu kwanga. ³¹ Mulungu na Tate wa Ambuye Yesu, wamene amatamandiwa ntawi yonse yosasila, aziba kuti ine sininama! ³² Pa Damasiko, kazembe osebenzela pansa pa Mfumu Aletasi anali ku londa muzinda waku Damasiko kuti anigwile ine. ³³ Koma bananiselusa ine kupitila mu basiketi kunipitisa pa zenela muchi bumba, nimwamene ine nina pulumusiwila mu manja yabo.

Chapter 12

¹ Lekani nizitukumule, koma kulibe nachamene ine nizapezamo. Koma nizakambapo pali vo-ona na vo-onesewa vohekela kuli Ambuye. ² Niziba muntu muli Kristu wamene zaka zokwanila makumi yanai na inai wamene-kaya kapena ni mutupi kapena anachoka mutupi, ichi ine siniziba, Mulungu ndiye wamene aziba-anatengewa kuyenda ku mwamba kwa chitatu. ³ Nafuti niziba kuti uyu mwamuna-kaya ngati ni mutupi, kapena anachoka mutupi, siniziba, koma Mulungu aziba- ⁴ anatengewa kuyenda ku Paladizo nakumvela vintu vamene vinali voyela kuti muntu avikambe. ⁵ Kuimililako uyu muntu nizazitukumula. Koma paine neka sinizazitukumula, koma pali chabe kufoka kwanga. ⁶ Ngati ine nasanka kuti nizitukumule, sinizankala chipuba, chifukwa nizankala nikamba cha zo-ona. Koma nizazichosako pa kuzitukumula, kuti osati muntu ali onse aniganizile kuchila mwamene nilili osati vamene aona kapena kumvela kuli ine. ⁷ Kutu nisazitukumule chifukwa cha kukulisa kwa vonilangisa, minga ina ikiwa mu tupi mwanga, kotumika na Satana kuti kanivutise-kuti nisankale ozitukumula maningi. ⁸ Katatu ninapapatila Ambuye pali ichi, kuti beve bakachosepo. ⁹ Koma anakamba kuli ine kuti, "chisomo changa nichokwanila pa umoyo wako, chifukwa mpavu zanga zima lengewa kunkala zofikapo ngati ndiwe ulibe mpavu." Chifukwa chake ine ningasankepo kuzitukumula pali kufoka kwanga, kuti mpavu za Kristu zingankale pali ine. ¹⁰ Chifukwa cha ichi ine ndine okutika chifukwa cha Kristu mu kufoka, kutukaniwa, muma vuto, mukuvutisiwa na mu ntawi zotaisa chikulupililo. Chifukwa ntawi yonse yamene ine nilibe mpavu, ndishi nili na mpavu. ¹¹ Ine nankala chipuba! Mwanikakamiza kuti nichite ichi, chifukwa ninali kufunika kuti nitamandiwe naimwe. Chifukwa sininali osalila kuli baja boitaniwa kuti niba tumiki bapa mwamba, ngakale kuti ndine wachabe. ¹² Volangisa kuti ine ndine mutumiki vinalangisiwa pakati panu mozigwila, vilangizo na vodabwisa na zintchito zampavu. ¹³ Nanga imwe munali munjila bwanji bochepekela kuchila zonse mipingo zina, kapema chabe kuti ise sitinali bokulemesani ise imwe? Munikululukile pali kulakwa uku! ¹⁴ Onani! Ine ndine okonzekela kuti nibwele kuli imwe ka chitatu. Sinizankala okulemesani imwe, chifukwa ine sinifuna vintu vamene vili nivanu. Nifuna imwe. Chifukwa bana sibafunika kusungila chuma makolo yabo. Koma, makolo ndiye bamene bayenela kusungila bana chuma. ¹⁵ Ine nizazipeleka mokondwela nakuzisebenzesa chifukwa cha myoyo zanu. ¹⁶ Koma monga mwamene chilili, sinina kulemelesani. Koma chifukwa chakuti ine ndine ochenjela, ndine wamene nakugwilani boza. ¹⁷ Kansi nanga imwe ine nina kusebenzesani kupitila muli muntu ali onse wamene ninatuma kuli imwe? ¹⁸ Ninalimbikisa Taitas kuti abwele kuli imwe, ndipo ninatuma na mubale wina pamozi na eve. Nanga Taitas anakusebenzesani kansi? Kansi sitina ende minjila imozi? ¹⁹ Kansi muganiza kuti ntawi yonse iyi tinali kuzi chingiliza ise kuli imwe? Pa menso pa Mulungu, muli Kristu tinali kukamba vonse kuti imwe munkale bolimba. ²⁰ Chifukwa ine niyopa kuti nikabwela ningakupezeni munjila yamene sinifuna. Niyopa kuti munganipeze kunkala muntu wamene simunali kuganizila. Niyopa kuti kungankale mukangano, kaduka, kuonekela kwa ukali, magulu, kunyozana, kukamba kumbali, ntota, na musokonezo. ²¹ Niyopa kuti ine nika bwela, Mulungu wanga anganichipese pakati panu. Niyo kuti ningafesesewe chifundo na bambili bamene banachimwa kumbuyo uku koma sibana tembenuke ku machimo yabo ya doti na uchiwelewele na zilako lako vamene banali kuchita.

Chapter 13

¹ Aka nika chitatu ine kubwela kuli imwe. "Kupasa muntu mulandu kuyenela kunkazikisisa na bamboni babili kapena batatu." ² Nakamba kudala pali abo bamene banachimwa kumbuyo uku nakuli bonse pamene ninali uko ka chibili, koma nizabwezapo nafuti: Pamene nizabwela nafuti, siniza balekelela. ³ Niku uzani ichi chifukwa chakuti mufuna funa umboni wakuti Kristu akamba kupitila muli ine. Eve siuja wamene alibe mpavu kuli imwe. Koma, niwa mpavu mukati mwanu. ⁴ Chifukwa eve anapachikiwa mopelebela mpavu, koma ali na moyo kamba ka mpavu za Mulungu. Chifukwa na ise ndise balibe mpavu muli eve, koma tinkala na moyo kamba ka mpavu za Mulungu pakati kanu. ⁵ Zipimeni pamweka, kuti muone ngati mukali mu chikulupililo. Ziyeseneni mweka. Nanga simuona paimwe mweka kuti, Yesu Kristu ali mukati mwanu?-Kapena, ngati, mwakangiwa mayeso. ⁶ Nipempela kuti muzaona kuti ise sitina kangiwe mayeso. ⁷ Manje ise tipempela kuli Mulungu kuti musachite chilchonse cholakwa. Sinipempela kuti tioneke monga tina pambana pama yeso. Koma, nipempela kuti muchite chintu chovomelezewa, ngakale kuti tioneke monga tinakangiwa mayeso. ⁸ Chifukwa sitingakwanise kuchita chilichonse choshusha va zo-ona, koma chabe kuvomelezana na va zo-ona. ⁹ Ise tikondwela pamene tinkala tilibe mpavu na pamene muli na mpavu imwe. Tipempela kuti munkale bofikapo. ¹⁰ Nilemba ivi vintu pamene ine nili kutali naimwe kuti pamene nipezeka naimwe nisaka muzuzule na ukali kusebenzesa mpavu zanga-yamene Ambuye bananipasa kuti niku kuliseni, osati kuku onongani. ¹¹ Posiliza, abale, kondwelani! Sebenzani pakubwezela, nkalani bolimbikisiwa, gwilisanani wina na munzake, nkalani mumutendere. Na Mulungu wa chikondi na mutendere azankala na imwe. ¹² Pasani moni ali onse na mpyompyono yoyela. ¹³ Bonse bantu ba Mulungu boyela bakupasani moni. ¹⁴ Chisomo cha Ambuye Yesu Kristu, chikondi cha Mulungu, na kupezekapo kwa Muzimu Oyela kunkale naimwe.

Galatians

Chapter 1

¹ Paulo, mutumwi- osati mutumwi ochokela ku munthu kapena kwa munthu nthambi, koma kuli Yesu Kristu ndi Mulungu Ambuye, amene anamuukitsa iye kuchokela kwakufa- ² ndiponso onse abale ndi ine, ku mipingo wa Galatiya: ³ Chikondi kwa inu ndiponso mutendere ochokela kwa Mulungu ndi Ambuye Yesu Kristu, ⁴ amene anazipatsa mwinewake chifukwa cha machimo yathu kuti iye anga timasule kuchokela ku chaka choophya, mogwilizana na chikonzekero cha Mulungu ndi Ambuye, ⁵ kuli iye khala ulemu nthawi ndi nthawi zonse. Amen. ⁶ Ine ndi odabwa kuti inu muli ku tembenukira kutali na iye wamene anamitanani pa chikondi cha Kristu. Ine ndi odabwa kuti inu muli kutembenukira ku mau amubaibulo osiyana. ⁷ Izi sikukamba kuti kuli wina mau amubaibulo, koma kuli ena anthu amene apangitsa inu mavuto ndiponso ali kufuna ku sintha mau amubaibulo ya Kristu. ⁸ Koma chingakhale ati ife kapena mungelo ochokela kumwamba ayenera ku chula kwa inu mau amubaibulo ena kuposa yamene tinachula kwa inu, lola iye ankhale wotembereredwa. ⁹ Ngati ife mwamene tinakamba pamaso, panopa ine nakamba kachiwili, " Ngati kuli amene alikuchula kwa inu mau ena kuposa amene inu munalandilila, lola iye ankhale wotembeledwa." ¹⁰ Pakuti kodi ndikopa anthu tsopano, kapena Mulungu? Kodi ndifuna kukoperetsa anthu? Ngati nilikukondweletsa anthu, sinizakakhala wanchito. ¹¹ Pakuti ndikudziwitsani inu, abale, kuti utenga wabwino wolalikila ndi ine suli monga mwa anthu. ¹² Ine sininaulandilekuchokela ku munthu, kapena sininaupunzile. Koma una bwela mwa bvumbulutso ya Yesu Kristu kuli ine. ¹³ Inu munamvela makhalidwe anga kale mwa chiyuda, mwamene ndinali kulondalonda mipingo wa Mulungu kupililila kuyesa ndiponso ine ninali kufuna kuyiononga. ¹⁴ Ndipo ndinawaposa ndi kutsogola mwa ciyuda ambiri a msinkhu wanga mwa mtundu wanga, ndipo neze wachangu kwambili ine ku miyambo zama nkolo anga. ¹⁵ Koma pamene Mulungu, amene anadipatula kuchokela mu mimba ya amai anga, ndiponso nakuniyitana mu cisomo cake, ¹⁶ kuti avumbulutse Mwana wake mwa ine, kuti ndimulalikile iye mwa amitundu, pomwepo sininafufumile kufunnsa thupi ndi magari. ¹⁷ Kapena kuyenda ku Yerusalemu kuli iwo amene anakhla atumwi pamene nikalimbe nkukhala ine. Koma ninayenda ku Arabiya ndipo ndinabwelanso ku Damasiko. ¹⁸ Pamenepo panapita zaka zitatu ndinapita ku Yerusalemu kuti nika muzibe Kefa ndiponso ine ninankhala kwa iye masiku khumi ndi asanu. ¹⁹ Koma wina wa atumwi sininamuone koma Yakobo, mbale wa Ambuye. ²⁰ Ndipo izi ndimilembelani inu, ine ndimilimbikitsani pamaso pa Mulungu, kuti sininama ine. ²¹ Pamenepo ndinabwela ku mbali za Suriya ndi Kilikiya. ²² Koma sinaliwozibika ku mipingo ya Yudeya amene alimu Kristu. ²³ Koma

amalinkumvela chabe kuti, " iye wakutilondalonda ife kale alikulalikila chikulupililo chamene anali chipasula kale." ²⁴ Ndipo analemekeza Mulungu chifukwa chaine.

Chapter 2

¹ Pamenepo pambuyo zaka ndi zina ndinabwelanso ku Yerusalemu pamodzi ndi Baranaba, ndinatengaso Tito kunipelekeza ine. ² Ine ndinayenda chifukwa chachi bvumbulutso ndiponso nina bauza uthenga wabwino wamene nilikulalikila kwa amitundu. Ine ndinalankhula mwamseri kuli ena amene anali olemkezeka, kuti kapena siningatamange- kapena sinatamange- chopanda phindu. ³ Koma angakhale Tito, amene anali ndi ine, ndiye Giriki, anamukakamiza kuti adulidwe. ⁴ Abale achiyengo anabwela mwa chisinsi kusuzumira pali ufulu wamene tilinawo mwa Kristu Yesu. Iwo anafunisisa kuti akatichitise ukapolo, ⁵ koma ife sitinakolola mwa kuzipeleka kuli iwo mu nthawi, kuti choonadi cha uthenga wabwino chingasale na inu. ⁶ Koma iwo amene anali kuonekela olemkezeka (chimene iwo anali kale, kulibe kanthu kwa ine, Mulungu samalangiza tsankho)- iwo, ine nakamba, amene analikuoneka olemkezeka sanawonjezele kanthu kalikonse kwa ine. ⁷ Poyamba mosiyana, iwo anawona kuti ine ndinapatsidwa na uthenga wa bwino kuli iwo amene osadulidwa, monga kwa Petro anapatsidwa uthenga wabwino wa mdulidwe. ⁸ Pakuti Mulungu anasebenza mwa Petro kumutuma kwa odulidwa, anachitanso mwa ine kundituma kwa amitundu. ⁹ Pamene Yokobo, Kefa, ndi Yohane, amene anazidikila kumanga mupingo, anamvetsa cisomo chamene ndinapatsidwa ine, iwo anapatsa ine ndi Barnaba dzinja lamanja la ciyanjano. Iwo anachita izi kuti ife tipite kwa amitundu, ndi iwo kwa mdulidwe. ¹⁰ Iwo anapempa kuti ife tikumbukile wosauka, ichichinthu chamene ine ndinali wofunisisa kuchichita. ¹¹ Koma pamene Kefa anabwela ku Antiokeya, ndinatsutsana naye pamanso pake chifukwa iye anatsutsika wolakwa. ¹² Pamanso wina wake anthu anabwela kuchokela kwa Yakobo, Kefa anali kudya ndi amitundu. Koma pamene aba anthu anabwela, iye anasiya ndipo anazipatula kwa amitundu. Iye anakuyopa iwo a ku mdulidwe. ¹³ Ndipo ayuda otsala anagwilizana mulizi za chinyengo. Ngankhale Barnaba anatengewa na chinyengocha iwo. ¹⁴ Koma pamene ine nina wona kuti machitidwe ya iwo sanali kuyenda mu choonadi cha uthenga wabwino, ndi nakamba kwa Kefa pamanso pa onse, " Ngati uli muyuda, koma munkhala monga amitundu ndipo si muyuda, mukangamiza bwanji amitundu kunkhala monga Ayuda?" ¹⁵ Ife tekha ndife Ayuda mwa chibadwile ndipo osati amitundu wochimwa; ¹⁶ koma ife tiziba kuti munthu sayesedwa wolungama pa nchito ya lamulo koma mwa chikulupililo cha Kristu Yesu. Ife tinabwela mu chikulupililo mwa Kristu Yesu kuti tikayesedwe olungama pa chikulupililo mwa Kristu ndipo osati panchito ya lamulo. Pa nchito ya lamulo kulibe thupi izayesedwa wolungama. ¹⁷ Koma ngati, pofuna kuyesedwa olungama mwa Kristu, tipezekanso tili ocimwa, kodi Kristu ama lengeza chimo? Simwamene nditu! ¹⁸ Ngati ine namanganso izi zintu zamene ninawononga, ine nazisimikizila ndekha ndine olakwa. ¹⁹ Pakuti mwa lamulo, kuti ine ndikhale ndi moyo kwa Mulungu. ²⁰ Ine ndinapacikidwa ndi Kristu. Sindine wamene alina umoyo ai, koma Kristu amene ali ndi moyo mwa ine. Koma moyo umene ndili nao mu thupi ndilinao mu chikulupililo cha Mwana wa Mulungu, amene ana ndikonda ndiponso nakuzipeleka chifukwa cha ine. ²¹ Ine sinimafaka pambali cisomo ca Mulungu, pakati ngati cilungamo cili mwa lamulo, nditu Kristu anafa pa chabe!

Chapter 3

¹ Agalatiya opusa! Kodi nidani amene afaka masenga pa inu? Panali pamaso pa inu pamene Kristu anaonetsedwa kupachikidwa. ² Ici cheka ndifuna kuphunzila kwa inu: kodi munalandila mzimu ndi nchito ya lamulo kapena ndi kumvela kwa cikhulupililo? ³ kodi iye ndi opusa? Popeza muzasiliza ndi thupi? ⁴ Kodi inu munavutika na zintu zambili kwa chabe- ngati poyenera anali kwa chabe? ⁵ Ndipo iye amene akupatsa inu mzimu ndi kusebenza nchito zamphamvu mwa inu, kodi ndi nchito za lamulo kapena ndi kumvela kwa cikhulupililo? ⁶ Monga Abrahamu anakhulupilila Mulungu ndipo kunalengedwa kwa iye cilungamo, ⁷ coteri zindikilani, kuti, iwo amene alinacikhulupililo ndi ana a Abrahamu. ⁸ Ndipo malembo, pakuoneratu kuti Mulungu adzayesa dungama amitundu ndi ndi cikhulupililo, anayamba kale kulalikila uthenga wa bwino kwa Abrahamu, kuti, "mwa iye mitundu yonse izadalisidwa." ⁹ Koteri kuti, iwo amene alina chikhulupililo. ¹⁰ Onse amene atama nchito za lamulo ali ndi tembelelo; ndiponso chinalebedwa, "wotembeledwa ali yense wosankhala m'zonse zintu zinalembedwa mubuku za lamulo, ndikuchita izi." ¹¹ Ndipo chinkhala koyera kuti kulibe ali yense wamene ayesedwa wolungama ndi lamulo pamaso pa Mulungu, chifukwa azankhala ndi moyo ndi chikhulupililo." ¹² Koma lamulo sichokela kwa chikhulupililo, koma munthu amene achita izi nchito za lamulo adzankhala ndi izi. ¹³ Kristu anatiombola ku tembelelo la chilamulo, pakunkhala tembelelo m'malo mwathu- pakuti mwalembedwa, "Wotembeledwa ali yense wopachika pamtengo"- ¹⁴ kuti dalitso la Abrahamu mwa Kristu Yesu lichitike kwa amitundu, kuti tikalandile lonjeza la Mzimba. ¹⁵ Abale, ndinena monga munthu. Pangano lingankhale la munthu, kulibe aliyense chabe, amene anga fake pambali kapena kuonjezalako, pamene yakukhazikila na lamulo. ¹⁶ Ndipo panopa malonjeza ananenedwa kwa Abrahamu ndi kwa mbeu yake. Sanena, " kwa zimbeu, ngati kunena zambili, koma kunena na imodzi, " ndipo kwa mbeu yako, " ndi ye Kristu. ¹⁷ Ndipo ichi ndinena: lamulo, limene linafika zinapita zaka mazana anai mphambu makumi atatu, pangano ya kukhazikika kale ndi Mulungu. ¹⁸ Pakuti ngati kulowa nyumba kuchokela kulamulo, sikuchokela kulonjezako. Koma Mulungu anapatsa Abrahamu kwa lonjezako. ¹⁹ Kodi, nanga, chinali cholinga cha lamulo? chinaonjezeka chifukwa cha zolakwa, kufikila mbeu ya Abrahamu amene analonjezela ndi angelo m'zanja la mkhalapati. ²⁰ Koma mkhalapati siliya imodzi, koma Mulungu ali modzi. ²¹ Kodi lamulo itsusana nao malonjezako a Mulungu? Iyayi simwanene nditu! Chifukwa ngati lamulo inapasiwa kuti ipase moyo, ndipo chilungamo sembe chinabwela na malamulo. ²² Koma malembo yanamanga machimo yonse. Mulungu anachita ichi pakuti lonjezo lopulumusa ise mwachikhulupililo muli Yesu ungapasiwe kuli bamene bakulupilila. ²³ Koma pamene chikhulupililo chikalibe kubwela, ife tinali wogwidwa mulamulo, mpaka chisomo china vumbulisidwa. ²⁴ Momwemo chilamulo chinakhala woyanganila mpaka kubwela kwa Kristu. Kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupililo. ²⁵ Koma popeza kuti chikhulupililo chabwela, sitinkhalanso muyansi a mkhalapakati. ²⁶ Pakuti inu onse muli ana a Mulungu mwa chikhulupililo cha mwa Kristu Yesu. ²⁷ Pakuti onse amene munabatizidwa kwa Kristu munavela Kristu. ²⁸ Muno mulibe myuda, kapena Greeki, muno mulibe kapolo, kapena omasuka, muno mulibe mwamuna ndi mkazi, pakuti muli onse mwa Kristu Yesu. ²⁹ Koma ngati muli a Kristu, inu muli mbeu za Abrahamu, nyumba monga mwa lonjezako.

Chapter 4

¹ Ine ndikunena kuti wolowa nyumba, akali mwana, sasiyana ndi kapolo, angankhale ndimwine waonse malowo onse. ² Koma iye ali pansi pa woyanganila ndi matrasiti mpaka tsiku yoikika kale ndi atate wake. ³ Koteru, pamene ife tikali ana, ife tinali akapolo ku miyambo ya dziko lapansi. ⁴ Koma pokwanilida nthawi, Mulungu anatuma Mwana wake, wobadwa ndi mkazi, wobadwa pansi la lamulo. ⁵ Iye anachita izi kuti aombole iwo amene anali pansi ya lamulo, kuti ife tikalandile kutenga ngati ana. ⁶ Ndipo chifukwa muli ana, Mulungu anatuma Mzimu wa Mwana wake alowe m'mtima zathu, amene amayitana, " Abba, Atate." ⁷ Koteru suli kapolo, koma mwana, koma ngati mwana, komanso inu ndi wolowa nyumba wa Mulungu. ⁸ Koma pa nthawi, pamene inu mukalibe kumuziba Mulungu, munapangiwa ukapolokuli iye, pa mphamvu zachilengedwe, osati milungu atonse. ⁹ Koma, manje kuti inu wabwela kuziba Mulungu, kapena ngakhale kuti inu munazibika ndi Mulungu, bwanji mubwelelanso ku miyambo zofoka ndi zopandaphindu? Kodi inu mufuna munkhale mu ukapolo chachiwili? ¹⁰ Inu musunga masiku, ndi miyezi, ndi nyengo, ndi zaka! ¹¹ Ndiopera inu kuti kapena nchito yanga nayinu kapena ndili yachabe chabe. ¹² Ndikupemphani inu, abale, khalani monga ine, pakuti ine nakhala monga inu. Simunanichitile choipa ine. ¹³ Koma inu muziba kuti nichifukwa chama tenda yathupi kuti ine ndinakhulalikani uthenga wabwino poyamba. ¹⁴ Ngakhale chiya cha m'thupi langa chakukuyesani inu, inu simunaninyoze kapena kunikana ine. Koma munandilandila ine monga mngelo wa Mulungu, monga ndine Kristu Yesu mwine. ¹⁵ Kodi pamenepo, dalitso lanu ili kuti? Pakuti ndikuchitilani umboni inu, kuti, ngati zotheka, inu mungabowole manso anu ndi kunipatsa ine. ¹⁶ Kodi nasanduka mdani wanu chifukwa nanena chonadi kwa inu? ¹⁷ Iwo alina changu pa inu, koma sivabwino ai. Iwo afuna kumivalani kunja inu, kuti inu mungankhale achangu kwa iwo. ¹⁸ Koma nichabwino kuchita changu muza bwino nthawi zonse, ndipo osati ngati nilipa modzi na inu. ¹⁹ Ana anga ochepa, kachiwili ine ndikukamba ndi kubeleka inu mpaka Kristu apangidwa mwa inu. ²⁰ Koma mwenzi ndinakhala nainu tsopano ndi kusintha mau anga, chifukwa ndi sinkhasinkha nainu. ²¹ Niuzeni ine, inu amene akufuna kunkhala omvela lamulo, kodi simukunva chilamulo? ²² Pakuti palembedwa kuti Abrahamu anali nao ana awili, mmodzi wobadwa kumusikana wa kapolo ndi mmodzi wobadwa kumkadzi wo masuka. ²³ Mmodzi anabadwa kumusikana wa kapolo monga mwa thupi, koma wina anabadwa kumkadzi womasuka mwa lonjezano. ²⁴ Izi zinthu zikutanthauza ziridwa ngati ndi zophiphilitsa, kuti akadzi aya ayimilila pazipangano ziwili. Mmodzi waku phiri la Sinai ndi akubalira ana ukapolo. ²⁵ Ndiye Hagara. Koma Hagara ndiye phiri la Sinai mu Arabiya; ndiponso iwo ndi Yerusalemu ya manje, pakuti ali muu kapolo pamodzi ndi ana ace. ²⁶ Koma Yerusalemu wa kumwamba ndiyo masuka, ndiponso ndiye amai atu. ²⁷ Pakuti kwalembedwa, "kondwela, osabala iwe,lila kunja ndipo kuwala kwa chisangalalo, inu wamene simuvutika naku wawa kwa kubala; chifukwa ana ali mbeta acuruka koposa iwo wa mkadzi amene alinaye mwamuna. ²⁸ Koma inu, abale, monga Isaki, tili ana a lonjezano. ²⁹ Koma ija nthawi iye wobadwa monga mwa thupi anazunza wobadwa monga mwa Mzimu. Ndiye chilili namanje. ³⁰ Koma lembo linena ciani? " Muchoseni musikana wa kapolo ndi mwana wake. Pakuti mwana wa musikana wa ukapolo sazalowa nyumba pamodzi ndi mwana wa mkazi womasuka." ³¹ Chifukwa cake, abale, ife sindise ana wa musikana wa ukapolo koma mkadzi womasuka.

Chapter 5

¹ Kristu anatisandutsa ufulu kuti tinkhale wa ufulu. Ima cholimba, chifukwa cake osati kuyikidwa kachiwili mugoli ya ukapolo. ² Onani, ine, Paulo, akunena kwa inu kuti ngati mwaleka amudulani, Kristu sazaka mipindulani inu mu kanthu. ³ Ndichitanso umboni kwa munthu onse wamene wolola amdule kuti iye ali wokakamizidwa kuchita vonse va mulamulo. Mulibe kanthu ndi Kristu, ⁴ inu amene muyesedwa olungama ndi lamulo; inu posiyana nacho cisomo. ⁵ Pakuti ife mwa Mzimu, kuchokela m'chikulupililo, tilindila chiyembekezo cha chilungamo. ⁶ Pakuti Kristu Yesu kapena mdulidwe kapena kusadulidwa chitantauza chilichonse, koma cikhulupililo chikusebenza mwa chikondi. ⁷ Inu munaliku tamanga bwino. Anakulesani ndani kuti musavele choonadi? ⁸ Uku kukakamiziwa sikuchokela kwa iye wamene anamitanani inu! ⁹ Ndiko chepa ka yisiti kamathandiza kupanga mkate onse wa mpala kuyima. ¹⁰ Ine ndikhulupilila mwa Ambuye kuti inu simudzankhala nao mtima wina. Koma iye amene akuvuta ni inu azaka lipila chilango, aliyense iye. ¹¹ Abale, ngati ine nikalikulalikilanso mdulidwe, chifukwa chani ine nikali ku imba mlandu? Pamenepo chikumudwitso ca mtunda wachosewapo. ¹² Ngati kuli ena amene akusogonezani inu, ine ndikafune kuti azi thena iwo! ¹³ Pakuti inu munayitanidwa ku ufulu, abale. Koma musacite wanu ufulu kuthandiza makhalidwe wolakwa; ngankhale, kondani ku pelekela wina ndi wina. ¹⁴ Pakuti mau amodzi akwanilisa chilamulo chonse ndiwo: " Inu konda muzako mwamene uzikonda." ¹⁵ Koma ngati iye mulumana ndi kudyana, chenjelani kuti iye simuna ankadya wina ndi wina. ¹⁶ Koma ndinena, yendani ndi Mzimu ndipo musafitse khumbila kwa thupi. ¹⁷ Pakuti khumbila kwa thupi kuli kusutsana na Mzimu, ndi khumbila wa Mzimu kuli kusutsana na thupi. Pakuti izi sizilingana, kuti zimene muzifuna musazicite. ¹⁸ Koma ngati musogolela ndi Mzimu, simuli pansi paulamulo. ¹⁹ Ndipo nchito za thupi zionekela: wachigololo chiwelewele, chodetsa, makhalidwe oipa, ²⁰ mafano, amatsenga, kuipa mtima, makangano, nsanje, zopsa ukali, kupikisana, malekano, magawano, ²¹ njiru, uchidakwa, woledzela chikondwelelo. Ndiponso zinthu monga izi. Ine ndiku chenjeza, mwamene ine ana chenjeza inu kale, kuti iwo amene alikuchita izi zinthu sazakhala ndi ndziko la Mulungu. ²² Koma chisepo cha Mzimu ndi chikondi, chisangalalo, mtendere, kusapupuluma, chikondi, chilungamo, cisomo, ²³ chifatso ndi kudzigwila; kuli izi zinthu kulibe lamulo. ²⁴ Iwo a Kristu Yesu anapachika thupi ndi zokhumba zake ndi khumbila. ²⁵ Ngati ife tinkhala mu Mzimu, tiyeni tiyende mu Mzimu. ²⁶ Osati tiyambe wodzikonda, phyetsa mtima wina ndi wina, njiru wina ndi wina.

Chapter 6

¹ Babale, ngati muthu agwiliwa mumachimo yena, emwe bamene mulipa muzimu muyenela kumubwezela mumuzimu motekanyila, kuti naimwe musayesewe. ² Nyamulilanani katundu wina ndi muzake, ndiponso mufikilize ma lamulo ya Kristhu ³ Ngati wina waimwe aganiza kuti ndine winawake angankale palibevamene alili, azinama eka. ⁴ Aliyense ayanganile nchito yake, pakuti ankale na lingo yozinvesela muli eve eka ndiponso osati mulimunzake. ⁵ chifukwa alionse azanyamula katundu yake eka. ⁶ Wamene aphunzisiwa mau ayenela kugabana zinthu zonse zabwino na wamene amuphunzisa. ⁷ Musanamidwe. Mulungu siamanamiwa, koma chilichonse chamene munthu ashanga, ndiye chamene azakolola. ⁸ Ndipo eve wamene ashanga mbeu kuuchimo wake, kuchokela kuuchimo wake azakolola chionongeko. Eve wamene ashanga mbeu ya ku muzimu, kuchokela kumuzimu azakolola umoyo osata kuchokela kumuzimu. ⁹ Tisafokele mukuchita zabwino, koma panthawi yoyenela tizakolola, ngati simugonjela. Ndiponso, pamene tili na danga, ¹⁰ tiyeni tichite zabwino ku munthu aliyense, makamaka abo bamunyumba ya chikulupililo. ¹¹ Onani malemba yakulu yamene nilembela kuli imwe na kwanja yanga. ¹² Iwo bamene bafuna kuzionesa munyama bayeselela kuoneka monga ni oduliwa. bamachita ivi kuyopakuti bangabavutise chifukwa chamutanda wa Kristhu. ¹³ Sichifukwa cha bamene banaduliwa beve beka kusunga lamulo, koma banafuna kuti imwe muduliwe pakuti bazinveselemo munkanda yao ¹⁴ Koma nisazinvese komachabe paza mutanda wa Yesu Kristhu mupulumusi, kupitila muziko lamene lina pachikiwa kuli ine, ndiponso kumaiko. ¹⁵ Pakuti siboduliwa kwamene kulengesa chilichonse olo kusaduliwa, koma chamene chilengesa nikunkala mwasopano muchilengedwe. ¹⁶ Kuli abobamene bakulupilila kulinganiza na chifuniro, cha mutendere ndiponso chifundo kunkala palibeve, napali Izilaeli ya Mulungu. ¹⁷ Kuchokela manjeapa kulibe anganivute, chifukwa ninyamula pathupi yanga zizindikilo za Yesu. ¹⁸ Chisomo cha Mbuye Yesu Kristhu chinkhala ndi muzimu wanu babale. Amen

Ephesians

Chapter 1

¹ Paulo, mutumiki wa Kristu Yesu mu chifunilo cha Mulungu, ku bantu boyela ba ku Aefeso, bokululupilika mwa Kristu Yesu. (Malembo yena ya Chi Giliki yalibe, Ku Efeso, koma kalata ioneka inatumiwa ku dera lameni li mu mapingo yasiyanasiyana, osati chabe mu Efeso). ² Chisomo kwainu na mutendere kuchokela kwa Mulungu Tate watu ndi Ambuye Yesu Kristu. ³ Mulungu ndi Tate wa Ambuye Yesu Kristu atamandiwe, wamene anatalisa na daliso ili yonse ya mu muzimu mu malo yaku mwamba mwa Kristu. ⁴ Mulungu anatisanka mwa eve kuchokela ku chiyambi cha ziko, kuti tinkale oyera ndipo balibe choipa pa manso pake. ⁵ Mulungu anatisankilatu poyamba kunkala bana bake kupitila mwa Yesu Kristu, kulingana nakukondwela kwa chifunilo chake. ⁶ Kulandiriwa kwatu kulengesa matamando ya ulemerelo wa chisomo chake chamene anatipasa chamahala mwa Iye Wamene Akonda. ⁷ Mwa Yesu Kristu tili nakuombolewa kupitila mu mwazi wake na kukululukiwa ma chimo yatu, kupitila mu kuchuluka kwa chisomo chake. ⁸ Anaikilapo maningi chisomo ichi paise mu nzelu zonse na kumvesesa konse. ⁹ Mulungu anachipanga chozibika kwaise kubisika kwa chifunilo chake, kupitila muli chamene china mukondwelesa, ndipo chamene analangiza mwa Kristu, ¹⁰ naichi na pamakonzedwe yofikila ntawi, kuleta zintu zonse pamozi, zintu ku mwamba na pansu, pa mutu umozi, ndipo Kristu. ¹¹ Mwa Kristu tinasankiwa mu cholowa chake, kukonzewelatu kulingana na pulani ya uyo wamene asebenza zonse kupitila na kukondwela kwa chifunilo chake. ¹² Mulungu anatisaka monga bo mupyana pakuti, ise bamene bali boyambila ku kulupila mwa Kristu, tinkale ba matandiwe pa ulemerelo wake. ¹³ Mwa Kristu, imwe namwe, pamene munanvela mau ya zoona, utenga wa chipulumuso chanu, munakulupilira mwa eve na kudindiwa na Muzimu Oyera wamene anakuchitani chipangano, ¹⁴ wamene ndi chizindikilo cha kupyana kwatu panka chiomboledwe chazintu, kukutamandiwa kwa ulemelelo wake. ¹⁵ Mwaichi, pamene ninanvela pa chikulupililo chanu mwa Ambuye Yesu na chikondi chanu cha banthu bonse ba Mulungu bo yera, ¹⁶ sinaleka kukamba zikomo kwa Mulungu chifukwa chaimwe pamene nikukambani imwe mu mapempelo yanga. ¹⁷ Nipempela kuti Mulungu wa Ambuye Yesu Kristu, Atate waulemelelo, azakupasani muzimu wa nzelu na chivumbuluso mu kumuziba eve. ¹⁸ Nipempela kuti manso amutima wanu achenjelesewe, kuti muzibe chikulupilo chamene anakuitinani ndi chitukuko cho pyanilapo cha ulemelelo wake pa banthu bonse ba Mulungu boyera. ¹⁹ Mumapempelo yanga nipempa kuti muzibe kusalinganisa kwa ukulu wa mpavu zake kwaise

okulupilira, kupitila mukusebenza kwa kulimba kwa mpavu zake. ²⁰ Izi ni mpavu zimozi zamene Mulungu anachita mwa Kristu pamene anamuusha kuchoka ku imfa nakumunkazika pa kwanja kwake kwa mpavu ku malo ya ku mwamba. ²¹ Anankazika Kristu patali ngako kuchila maulamulilo ndi kulinganila ndi mpavu ndi ndime, ndi zina lonse linga kambiwe. Kristu azalamulila, osati chabe mu ntawi iyi, koma na mu ntawi yamene ibwela. ²² Mulungu Anaika zintu zonse mukunvelela pansi pa mendo ya Kristu nakumupasa mupingo ankale mutu wa zinthu zonse. ²³ Mupingo ni tupi yake, kukwanilisika kwa iye wamene akwanisa zonse mwa zonse.

Chapter 2

^{1 2 3} Ndipo inu, mwenzeli bakufa muzolakwa zanu na mumachimo yanu, zimene munayendamo, kulingana na ntawi ya ziko iyi. Mwenzo onkala kulinganiza na mukulu wa ma ulamulilo ya mu lengalenga, muzimu wamene usebenza mubana bosanvelela. Pa ntawi ina bonse tinankalapo na aba banthu, kufikilizisa zifunilo zoipa za matupi yatu, ndipo kuchita zifunilo za tupi na maganizo yake. Tenzeli mwachibadwire bana baukwiyo munga banthu bena bonse. ⁴ Koma Mulungu niolemela mu chifundo chifukwa cha chikondi chake chikulu chamene anatikondera ise. ⁵ Pamene tenzeli bokufa mu kulakwa, anatilenga umoyo pomozi mwa Kristu – mu chisomo munapulumusika. Mulungu anatiusha pamozi na Kristu, ⁶ ndipo Mulungu anatipanga kunkala pamozi ku malo ya kumwamba mwa Krsitu Yesu, ⁷ pakuti mumanyengo yali kuza akalangize kwaise chuma chosapenda chikulu cha chisomo chake chamene analangiza mukukoma mutima kwake kwaise mwa Kristu Yesu. ⁸ Chifukwa mwa chisomo munapulumusika kupitila muchikulupiliro, ndipo ichi sichinachoke kwa inu, ni mpatso ya Mulungu, ⁹ yosachoka kuzochita, pakuti wina asazitukumule. ¹⁰ Chifukwa ndise bopangiwa ba Mulungu, bopangiwa mwa Kristu Yesu kuchita nchito za bwino zamene Mulungu anapangilatu kwaise, kuti tikayendere mwamenemo. ¹¹ Chomwecho kumbukani kuti pa ntawi ina mwenzeli bakunja mu tupi. Muitaniwa “bosadulidwa” naicho chamene chiyitanidwa “chodulidwa” mu tupi yopangiwa na manja ya banthu. ¹² Chifukwa pa ntawi ija mwenzeli bochosewako kuli Kristu, alendo kudera la Yisraeli, osazibikwa ku mupangano wa malonjezano, bopanda chiyembekezo ndipo bopanda Mulungu mu ziko ili. ¹³ Manje mwa Kristu Yesu inu bamene benzeli kutali na Mulungu munabwezewa pafuti na gazi ya Kristu. ¹⁴ Chifukwa ndiye mutendere wathu. Anapanga babili umozi. Kupitila mu tupi yake anagumula khoma lochinga pakati kaife. ¹⁵ Nikuti, anachosako udani na lamulo pakuti alenge muntu umozi wa sopano mwaeve, ndipo kupanga mutendere. ¹⁶ Kristu anayanjanisa banthu babiri mu tupi imozi kwa Mulungu kupitila mu mutanda, kupaya udaniwo. ¹⁷ Yesu anabwera nakulalika utenga wabwino wa mutendere kwa inu bamene benzeli kutali na mutendere kwa abo benzeli pafuti. ¹⁸ Chifukwa kupitila mwa Yesu bonse babiri tili namulowedwe mwa Muzimu omozi kwa Atate. ¹⁹ Sopano, manje imwe bakunja sindimwe balendo ndi bobwera cahbe. Koma ndimwe banthu bamuziko imozi na bantu boyera ba Mulungu ndipo bana ba nyumba ya Mulungu. ²⁰ Munamangidwa pa ziko ya batumwi ndi aneneri, ndipo Kristu Yesu wamene ndiye mwala wa pangodya. ²¹ Mwaeve mumangidwe onse wankala olumikizika pamozi bwino ndipo ukula kunkala tempele yoyera mwa Ambuye. ²² Nimwaeve mwamene naimwe mumangidwa pamozi munga malo yonkalapo Mulungu mu Muzimu.

Chapter 3

¹ Chifukwa chaichi ine, Paulo, ndine kaili wa Kristu chifukwa chainu bakunja. ² Nizindikila kuti munanvela kusebenza kwa chisomo cha Mulungu chamene chinapasiwa kwaine chifukwa chanu. ³ Nilemba kuzindikila na chivumbuluso chinaoneka kwaine. Ichi nichazoona chobisika chamene ninakulembelani inu mwachichepele. ⁴ Pamene mubelenga pa ichi, muzankala oziba mushe kuziba kwanga kwaichi chonadi chobisika pali Yesu. ⁵ Mumabadwire yena ichi chonadi sichenze chozibisiwa ku bana ba banthu. Koma manje nichovumbulusiwa na Muzimu ku ba tumiki bake ndi baneneri bake. ⁶ Ichi chobisika chazoona nichakuti banthu bakunja bazalowa pamozi na ise, ndipo ni banthu ba tupi imozi ndipo bankala kudyamo mu chipangano cha Kristu Yesu kupitila mu utenga. ⁷ Ngati ninankala kapolo wa utenga kupitila mu mpatso ya chisomo cha Mulungu chinapasidwa kwaine kupitila mukusebenza kwa mpavu zak ⁸ Kwaine – olo ndine wachichepele wapansi pa banthu bonse boyera ba Mulungu – ichi chisomo chinapasiwa, kupeleka utenga ku Bakunja chuma chosasindikila cha Kristu ⁹ ndi kuleta kuwala kwa onse pa pulani – kubisika kwamabadwire mwa Mulungu, wamene anapanga zintu zonse. ¹⁰ Iyi pulani inaululidwa kupitila mu mupingo pakuti bakulu na balamulili mu malo yaku mwamba bangabwere kuziba mapangidwe yosiyanasiyan ya nzelu za Mulungu. ¹¹ Ichi chinachitika kulingana na pulani yosata yamene anakwanisila mwa Kristu Yesu Mbuye watu. ¹² Chifukwa mwa Kristu tili na kulimba ndipo tingena na chizindikilo chifukwa cha chikulupiliro chatu mwaeve. ¹³ Nichamene ni kupempani kuti musabwezewa mitima pansi chifukwa cha mavuto yanga pa imwe, chamene ni cha ulemelelo wanu. ¹⁴ Mwaichi nigwadisa makufi yanga kwa Tate, ¹⁵ kwamene banja yonse ku mwamba na pa ziko inapasiwa zina. ¹⁶ Nipempela kuti angakupaseni, kuyanira na chuma chake mu ulemelelo, kuti mulimbisiwe na mpavu kupitila mu Muzimu, wamene uli mukati kanu. ¹⁷ Nipempela kuti Kristu ankale mu mitima zanu kupitila mu kukulupilira, na mizu zanu ndi ziko mu chikondi, ¹⁸ pakuti munkale boziba mushe, pamozi nabantu bonse boyenera ba Mulungu, makulidwe, ndi ntafu, ndikulepa, nakusika, ¹⁹ ndikuziba chikondi cha Kristu, chamene chipitilila kuziba, pakuti muzule nakufikapo kwa Mulungu. ²⁰ Manje kwaeve wamene ali na mpavu zochita kuchilapo zonse zamene tipempa ndi kuganiza, kupitila mu mpavu zake zamene zisebenza mwaise, ²¹ kwaeve kunkale ulemelelo mu mupingo na mwa Kristu Yesu ku mabadwire yonse masiku yosata. Amen.

Chapter 4

¹ Ndipo, ine munga omangiwa chifukwa cha Ambuye, nikulimbikisani kuti muziyenda mo yenera na mwamene munaitaniwa. ² Nikulimbikisani kuti muzinkala bozichepesa maningi ndipo bo teka mitima nakutekanya, ndikugwilizana umozi ndi muzake mu chikondi. ³ Chitani motero kuti musunge kugwilana kwa Muzimu ndi kulimba kwa mutendere. ⁴ Kuli tupi imozi na Muzimu Umozi, munga mwamene munaitaniwa mu kukulupirila kwa ma maitanidwe yanu. ⁵ Ndipo kuli Ambuye umozi, chikulupiliro chimozi, na kubatiziwa kumozi, ⁶ ndipo Mulungu umozi na Tate wa bonse, wamene ayanginila vonse ndipo kupitila muli vonse na muli bonse. ⁷ Kwaise bonse wina na wina kunapasiwa chisomo kulinganiza na mpatso ya Kristu. ⁸ Chilimonga mwamene malembedwe yakamba: “pamene anakwezeka ku mwamba, anangenesa kumangiwa mu kumangiwa, ndipo anapasa mpatso ku bantu.” ⁹ Kodi chitantaucha chani kuti “anakwezeka” koma ngati anabwera pa madera ya pansi ya muziko? ¹⁰ Wamene anabwera ni umozi muntu wamene anakwezeka ku mwamba maningi kuchila mulengalenga, kuti akwanilise zintu zonse. ¹¹ Kristu anapasa bena kunkala ba tumwi, ndipo bena aneneri, ndipo bena balaliki, ndibena ma busa na bapunzisi. ¹² Anapasa nchinto izi kuti balimbise bantu ba Mulungu kuchita chinto zo sebenza, kumanga tupi ya Kristu. ¹³ Apitiliza kumanga tupi yake panka bonse tikafike kugwilana kwa chikulupiliro na kuziba Mwana wa Mulungu, ndipo kuti tinkale bokula na kufikila kuchipimo chamakulidwe ya Kristu. ¹⁴ Kristu atimanga ise pakuti tisankale munga bana bong’ono botaiwa uko na uko na miza, otengewa na miza za mapunziso ndipo za bantu bo nyenga mu manyengo yabo yaboza. ¹⁵ Koma, kukamba zoonza mu chikondi, tizakula munjila zonse mwa iye wamene ni mutu, ndipo, Kristu. ¹⁶ Kristu amanga tupi yonse, ndipo inayikiwa na kugwilana pamozi na mizipe, ndipo yasebenzela pamozi, manje pamene pati yina ndiyinzake vasebenzela pamozi, ichi chilengesa tupi kukula pakuti ingazimange yeka mu chikondi. ¹⁷ Nichomwecho, nikamba ndipo nifotokoza paizi mwa Ambuye, kuti masaziyenda munga mwamene bakunja bamayendela, mu kupusa kwa mu mitu zabo. ¹⁸ Balinamudimu mu kuziba kwabo, nibochosewako ku umoyo wa Mulungu chifukwa chakusaziba kwamene kuli muli beve, chifukwa chamitima zabo zolimba. ¹⁹ Banankala balibe nsoni ndipo banazipeleka beka ku chiwelewele, ndipo bamachita machitidwe ya madoti mukuzikonda. ²⁰ Koma simwamene munapunzila pali Kristu. ²¹ Niziba kuti munanvela pali eve, ndipo muna punzisiwa mwa eve, munga mwamene chonadi chili mwa Yesu. ²² Munapunzisiwa kuchosa za mankalidwe yakudala, kuchosako munthu wakudala. Ni munthu wakudala wamene ali nabumambala chifukwa chazifunilo zake zo nyenga. ²³ Munapunzisiwa ku sukiwa muzimu wa maganizo yanu, ²⁴ ndipo kuvala munthu wa sopano wopangiwa mu chionekela cha Mulungu – mukudera na kuyenera kwa zoonza. ²⁵ Nichomwecho, tayani maboza, ndipo lekani alionse akambe zoonza ku munzake, chifukwa ndimwe banja imozi. ²⁶ Kwiyani koma musachimwe. Musaleke zuba igwele pa ku kwiya kwanu. ²⁷ Musapase mujelekezi ndime. ²⁸ Wamene enze kuba asabe futi. Koma, afunika kusebenza, kusebenzela pa za bwino na manja yake, pakuti angankale na chopasa banzake balibe kantu kalikonse. ²⁹ Musaleke kukamba kwachionenge kulikonse kuchoke mu kanwa kanu. Sebenzesana chabe mau ya bwino yamene yazaleta chilimbiso kwa aba bamene bachifunisisa, pakuti mau yanu yalete chisomo kwa abo bamene bayanvela, ³⁰ Ndipo musachite chliliso kwa Muzimu Oyera wa Mulungu, chifukwa ndimwe eve mwamene munachitiwa chidindo cha pa siku ya Chipulumuso. ³¹ Tayani kuzivuta mitima konse, ukali, kukwiya, kushautana, ma nyozo, ndi zintu zonse zoyipa. ³² Nkalani na chikondi ku wina ndi munzake, munkale na mitima zamushe, kukulukililana, mwamene Mulungu anakukulukililani mwa Yesu Kristu.

Chapter 5

¹ Nichomwecho nkalani bokonkeleza Mulungu, monga bana bokondewa. ² Ndipo yendani muchikondi, mwamene naeve Yesu anatikonda nakuzipeleka eka kwaise. ³ Koma pasankale dama iliyonse painu ya ma chimo ya chiwelewele kapena chisiliro olo chidetso, chifukwa ivi nivosayenera pa bantu ba Mulungu boyera. ⁴ Lekani pasankale chinyaso, kapena kukamba kopusa, ndipo pasankale majokusi yosayenera – ivi vonse sivifunika. Koma pankale kupeleka mayamiko. ⁵ Chifukwa muziba ndipo muzindikila kuti kulibe aliyense wamene achita chiwelewele, wachideso, kapena wosilira – uyu munthu wopempeza tumilungu twina – azalowa mu Ufumu wa Kristu ndi Mulungu. ⁶ Musaleke aliyense akunameni na mau yopanda pindu, chifukwa chaizi zintu ukwiyo wa Mulungu ubwera pa bana bosanvelela. ⁷ Nichifukwa chake, musankale olandirana nabo. ⁸ Chifukwa mwenzepo mudimu, koma manje ndimwe kuwanika mwa Ambuye. Yendani monga bana bachiyaniko ⁹ (chifukwa zopeleka za kuwanika zipezeka mu ubwino onse, kulungama, na mu chonadi), ¹⁰ ndipo punzilani chamene chisekesa Ambuye. ¹¹ Musayanjane na nchito zilibe pindu za mudimu, koma muzisuse. ¹² Chifukwa sichoyana nakukambapo zintu zamene bamachita museri. ¹³ Koma pamene chintu chaululidwa mu kuwunika, chimaonekela. ¹⁴ Chifukwa chonse chamene chionekela nikuwanika. Chomwecho chikambiwa, “wuka, iwe wogona, ndipo ima kuchoka ku imfa, ndipo Kristu azawala pa iwe.” ¹⁵ Onani mushe mwamene muyendera – osati monga balibe nzelu koma ngaba nzelu. ¹⁶ Mubwezelepo ntawi chifukwa masiku niyoipa. ¹⁷ Chomwecho, musankale bopusa, koma zibani chifunilo cha Ambuye. ¹⁸ ²⁰ Musakolewe na vinyo, chifukwa ichi chiipeleka kumachitidwe yotayika. Koma, nkalani ozula na Muzimu Oyera, ¹⁹ kukambisana mu masalimu ndi ma himino ndi nyimbo za uzimu, kuyimba ndi kukomesera kwa Ambuye na mutima wanu onse, ²¹ Ndikupeleka mayamiko pa zonse muzina la Ambuye Yesu Kristu kuli Mulungu Tate, na kunvelelana wina ndi muzake mukoyopa Kristu. ²² Bakazi, nvelelani bamuna banu, monga ni kwa Ambuye. ²³ Chifukwa mwamuna ndiye mutu wa mukazi monga Kristu naye ni mutu wa mupingo, wamene mupulumusi wa tupi. ²⁴ Koma mwamene mupingo unvelela Kristu, bakazi nabo banvelele bamuna babo mwa zonse. ²⁵ Bamuna, kondani bakazi banu, mwamene Kristu anakondela mupingo ndi kuzipeleka eka mumalo mwake pakuti akaupatule, ²⁶ anauwamya ndi ku usuka na manzi na mau, ²⁷ pakuti angazipase eka mupingo wa ulemelero, wopanda banga, kapena kwinya, kapena kanthu kotere, koma oyera ndiopanda chilema. ²⁸ Munjila imozi bamuna bafunika kukonda bakazi babo monga matupi yabo. Wamene akonda mukazi wake azikonda eka nae. ²⁹ Chifukwa kulibe muntu wamene anazondapo tupi yake, koma amaidyesa bwino na kuzisunga bwino, monga mwamene Kristu adyesela na kusunga bwino mupingo, ³⁰ chifukwa ise ndise ziwalo za tupi yake. ³¹ “Chifukwa chaichi mwamuna azasiya tate wake ndi mayi wake ndipo azapatikizana ku mukazi wake, ndipo aba babiri bazankala tupi imozi.” ³² Ichi chonadi chobisika nichikulu – koma nilikulankula pa nkani ya Kristu ndi mupingo. ³³ Komanso, aliyense pa inu afunika kukonda mukazi wake monga mwamene azikondela, na mukazi apase ulemu mwamuna wake.

Chapter 6

¹ Bana, nvelelani makoro anu mwa Ambuye, chifukwa ichi nichabwino. ² "Lemekeza tate wako ndi mayi" (ili ndiye lamulo loyamba lonkala nachilonjezano), ³ "pakuti zinthu zizikuyendela mushe ndipo unkale ntawi ikulu pa ziko." ⁴ Atate, musakwiye bana banu. Koma, mubakulise mukuzilela na muchilangizo cha Ambuye. ⁵ Bakapolo, muzinvelela ma bwana yanu akutupi na ulemu ukulu ndi kuyopa, ndi mutima wanu osakumbukira kanthu kena. ⁶ Banveleleni mwameni munganvelele Kristu. Musanvelele chabe pamene ma bwana yanu yakali kumiyangana, pakuti mubanvese mushe. Koma, munvelele monga bakapolo ba Kristu, bamene bachita chifunilo cha Mulungu kuchoka mu mutima wanu. ⁷ Sebenzani namitima zanu zonse, monga musebenzela Ambuye osati banthu, ⁸ chifukwa tiziba kuti chilichonse chabwino chamene wina achita, chizalandila chobwezela kwa Ambuye, angankale ni kapolo kapena omasuka. ⁹ Mabwana, nainu mubachitile zinthu zomwezo iwo. Musabanyoze. Muziba kuti iye wamene ali Mbuye wabo ndi inu ali ku mwamba, ndipo kulibe sanku kwa iye. ¹⁰ Chosalira, limbani mwa Ambuye ndi mu mukulimba kwa mpavu zake. ¹¹ Valani chovala cha usilika cha Mulungu, pakuti mukalimbe pa muchenjelelo wa mujelekezi. ¹² Chifukwa kulimbana kwatu sikulimbana kwa mutupi na gazi, koma tilimbana na maukulu, ndipo na maulamulilo, na ma mpavu ya aziko lino la mudimu, na mpavu za mizimu zoipa umo mu malo yaku mulengalenga. ¹³ Mwaichi valani chovala chomenya ngondo ya Mulungu, pakuti mukaimilile pa siku ya mayeso, ndipo mukasilizisa kuchita zonse, mukankale bolimba. ¹⁴ Nkalani bolimba, zimangileni muchuwuno mwanu na chonadi, muvalenso chapachifuwa chachilungamo, ¹⁵ ndipo, na mendo yanu yankale nakuzipeleka kwamene kuchokela ku utenga wa mutendere. ¹⁶ Mulivonse vamene mupitamo tengani chikopa chachikulupiliro, chamenecho muzazimila mivi yonse yoyaka moto ya muntu oyipa. ¹⁷ Ndipo tengani chisote chachiulumuso na lupanga lwa Muzimu, lyamene luli ndi mau ya Mulungu. ¹⁸ Napempelo lonse ndi pempezero, pempelani ntawi zonse mu Muzimu. Mukusilizisa, muziyanganila na kulimba konse pamene mupeleka ma pempelelo yanu pa banthu bonse boyera ba Mulungu. ¹⁹ nipempeleleni koni naine, kuti mau yapasiwe kwaine pamene nili kusegula kamwa kanga. Pempelelo kuti nilangize mu kulimbikisa chonadi chobisika pa nkani ya utenga. ²⁰ Nichifukwa cha utenga chamene ndiri kazembe omangiwa mu unyolo, pakuti nilankule molimbika, mwamene nifunika kulankulila. ²¹ Tayichikas, mubale wokondewa ndi kapolo wachendi mwa Kristu, azakuuzani zonse, pakuti muzibe mwamene nilili. ²² Namutuma kwainu chifukwa cha chamene ichi, pakuti muzibe mwamene tilili, ndipo pakuti alimbikise mitima zanu. ²³ Mutendere kwainu ba bale, ndi chikondi na chikulupiliro kuchokela kuli Mulungu Tate ndi Ambuye Yesu Kristu. ²⁴ Chisomo kwainu monse bamene mukonda Ambuye watu Yesu Kristu na chikondi cholimba ngako.

Philippians

Chapter 1

¹ paulo na Timoteyo akapolo ba Yesu Christu kwa bonse bamene bana itanidwa,kwa bonse banaitaniwa na Yesu.Yesu wamene ku Philipo na onse woyanganila nama Diconi. ² Chisomo chinkale na imwe na mtendere kuchokela kwa Mulungu atate bathu nakuli Yesu Christu. ³ Niyamikila Mulungu pamene nimamukumbukilani. ⁴ Nthawi zonse,kumukumbukilani mumapempelo, ⁵ Nimapempela nachimwemwe.Nimayakila futi kamba ka kubwela pamozi kwathu kuchokela siku yoyamba kufikila manje. ⁶ Nili na chisimukizo kuti wamene anayamba ntchito yabwino muli imwe azaisiliza kufikila siku ya Yesu Christu. ⁷ Nichabwino kuti inemvele mwamene nimvelela pali imwe kamba kakuti monse muli Mmtima mwanga.monse mwankala osebenza naine muchisom namndende namuchisimikizo cha uthenga. Pakuti Mulungu anachitila umboni ⁸ kuti nifunisisa monse imwe nachifundo mwa Yesu Christu. ⁹ Ine nipempelela ichi'kuti chikondi chanu chikulileko nakuti mukule mukuziba nakumvesesa. ¹⁰ Nipempelela ichi kuti muzibe chabwino nakuti munkahle olungama,osankhala nachoipa pasiku ys Yesu. ¹¹ Nimupempelelani kuti muzazula na chipaso chachiyelo chamene chibwela na Yesu Christu,kuulemelo nakuyamikila Mulungu. ¹² Nifuna kuti muzibe abale kuti vamene vachitika kuli ine vachitikila kuti kulalikila kwa mau kupite pasogolo. ¹³ Kamba ichi kumangiwa kwanga kunaonekela poyera kuli aliyense kwa olonda ku nyumba yachifumu nakuli wanangu aliyense. ¹⁴ Ambili abale alichu chisimikizo mwa ambuye kamba ka unyolo wamene nilimo,ndipo balifuti balalikila mau mopanda mantha. ¹⁵ Benangu balalikila Yesu na mitima ya nsanje nandeo,bena balalikila mau na lingo yabwino ¹⁶ Aba bachibili balalikila mau mwachikondi kuziba kuti ninaikiwa pano kuti nikadifende uthenga. ¹⁷ Ao benangu balalikila mau nalingo yaipa,osati yabwino.Baganiza kuti

bazaninzunza pamene nili mu unyolo. ¹⁸ Nichani manje?Nikongukuti munjila iliyonse,muboza kapena muchoonadi Yesu alalikiwa ndipo mwaichi nisangalala,Inde nizasangalala. ¹⁹ Chifukwa niziba kuti ichi chizaleta kumasukwa kwanga kupitila mumapempelo yanu na thandizo ya Muzimu Oyera wa Yesu Christu. ²⁰ Nikulingana na chiyembekezo changa chakuya na chiyembekezo chinangu kuti sinizamnvesedwa manyazi,ndipo nakulimba mtima konse monga mwa nthawi zonse, Yesu azakwezedwa muthupi yanga,mu umoyo kapena imfa, ²¹ Kwa ine kunkhala na moyo Ni Yesu,ndipo nikafa ninshi naphindula. ²² Koma ngati nikunkhala muthupi,chitantauza kupeza bwino mukusebenza kwanga.koma nizasobesa chani? Siniziba. ²³ Chifukwa ine napezeka opsyinga pakati pali vibili.kufuna kwanga nikuyenda kwa Yesu chapene nichabwino, ²⁴ koma kunkhala muthupi nichabwino kuli imwe, ²⁵ kusimikizila ichi niziba kuti nizankhala ndipo nizapitiliza kunkhala naimwe monse. ²⁶ kuti mukazipitilila pasogolo namu chimwemwe chamchikhulupililo.kuti mwaine munkale na zifukwa zopitilila zonyadila mwa Yesu Christu nikayenda kubwela futi kuli imwe. ²⁷ Koma mankalidwe yanu yankale yoyenera mu uthenga wa Yesu Christu,chakuti nabwela kapena siniliko,nikamvele kuti imwe muimilila nganganaga mumuzimu umozi,nzelu zimozi,pamozi kuyesesa muchikhulupilo cha uthenga. ²⁸ Asamuchitiseni mantha munjila iliyonse kuli bamene bamususani.Ichi nichioneselo chachiwonongeko chao,koma nichipulumuso chanu,elo ichi chichokela kwa Mulungu. ²⁹ Pakuti kuli imwe chinapasiwa mwa Yesu Christu,osati kungokhulupilila chabe eve,koma nakuvutika mulieve. ³⁰ Kunkala na mukangano wamene munaona muli ine ndipo muunvela kuli ine.

Chapter 2

¹ Ngati pali chilimbikiso chilichonse mwa Christu,ngati pali chitonthozo kuchokela muchikondi,ngati pali chiyanjano cha muzimu,ngati pali chifundo na kuwama, ² mufikilise chimwemwe changa pakugani pali ivi,kunkala nachikondi chimozi,kunkala ogwilizana mwa Yesu,nakunkala na lingo imozi. ³ musachite chilichonse mwanjilu kapena palibe kanthu,koma mozichepesa muganizile benangu kunkala bwini kuchila imwe. ⁴ Wina aliyense asasamalile vofuna zake koma,koma vofuna zabanzake. ⁵ Muganize munjila yamene inali mwa Yesu Christu. ⁶ Anakhala muchifanizilo cha Mulungu,koma sanaziyese kulingana na Mulungu,ngati chinthu chogwilililako. ⁷ Koma azachosa zonse zenze mulieve,nakuzipanga ukapolo.Anaoneka muchifanizilo cha munthu.Anapezeka namaonekedwe ya munthu. ⁸ Anazichepesa nakugonjela kufikila ku imfa,nga ⁹ Ndipo Mulungu anamkweza eve maningi.Anamupasa zina yopambana mazina yonse. ¹⁰ Anachita ichi kuti muzina ya Yesu bondo iliyonse ikalambile,bondo ya onse alikumwamba,alipaziko ya pansi na awo ali pansi pa ziko ya pansi. ¹¹ Anachita ichi kuti lilime iliyonse ikavomekeze kuti Yesu Christu ni Mfumu ku ulemelelo wa Mulungu tate. ¹² Abale mwamene mwankhala mulikumnvelela nthawi zonse,osati chabe pamene nilipo,koma manje kwambili pamene sinilipo,musebenzele chipulumuso chanu mwa mantha nakunjenjema. ¹³ Chifukwa ni Mulungu wamene asebenza mwai imwe kuti mufune nakuchita zabwino kwa eve. ¹⁴ Chitani vinthu vonse mosadandaula nakuchita ndale. ¹⁵ Muchite telo kuti winangu asamupezeni na choipa nakuti munkhale olungama,Bana alibe choipa.Munkhale tele kuti mukawale monga nyali muziko,pakti pa banthu oipa na mubadwo otaika. ¹⁶ Mugwilisise mau ya moyo kuti nikankhala nayo danga yakuulemelelo pasiku ya Christu.Ndiye pamene nizaziba kuti sininathamange pachabe kapena kusebenza pachabe. ¹⁷ Koma olo kuti napekelewa monga nsembe pa chopeleka na kusebenza kwa chikhulupililo chanu,Nisangalala,elo nisangalala naimwe monse. ¹⁸ Munjila imozi naimwe musangalale,elo musangalale naine. ¹⁹ Koma niyembekezela mwa Yesu Christu kumutumizilani Timoteyo kwa imwe manjemanje kuti naine nikalimbisidwe pamene nizaziba vinthu pali imwe. ²⁰ Pakuti nilibe winangu aliyense wamene alina kulakalaka monga eve,wamene afunisisa imwe. ²¹ Pakuti onse amafuna zofuna zao,osati zofuna za Yesu Christu. ²² Koma muziba mtengo wake,kuti mwamene mwana atumikila atate bake,motelo atumikila naine muuthenga. ²³ Niyembekezela kumutumiza kwa imwe kulinga mwamene vinthu vizayendela naine.

²⁴ Koma nilinacho chisimikizo mwa Ambuye kuti ine naine nizabwela kwaimwe manje manje. ²⁵ Koma niganiza kuti nichoyenera kutumiza Epaphroditus kuti abwelele kwa imwe.Nimubale wanga nanchitho mnzanga,namusilikali mnzanga,ndipo nimutumiki wanu,kapolo wa zofuna zanga. ²⁶ Pakuti anavutisiwa,nakufunisisa kunkhala na imwe monse,chifukwa munamvela kuti enze odwala. ²⁷ Pakuti Anadwalisa maningi chakuti sembe anafa.Koma Mulungu anamuchitila chifundo,osati eve eka,koma naine kuti nisankhale namabvuto pamabvuto. ²⁸ Nichabwino maningi kuti nimutumiza kuli imwe,kuti mukamuona futi,kuti musangalale kuti ine nimasuke kuvodandaula. ²⁹ Landilani Epaphroditus nachimwemwe chonse.Pasani ulemu banthu monga uyo. ³⁰ Pakuti kenze kamba ka ntchito ya Yesu kuti anali pafupi nakufa.Anapeleka moyo wake kutumikila ine

Chapter 3

¹ Posilizila, abale,Sangalalani mwa Ambuye.Kwa ine kumulembelani ivi vinthu nafuti sikumusokonezani.Ivi vinthu vizakusungani otetezedwa.Munnkhale menso kuona imbwa.Nkhalani menso nasebenza azoipa. ² Nkhalani menso kuli bamudulidwe. ³ Pakuti ndise bamudulidwe.Ndise amene tipembeza mumuzimu wa Mulungu.Ndise amene timekela mwa Yesu Christu,ndipo sitimekela mthupi. ⁴ Kunkhala telo naine ningadalile mthupi.Ngati winangu adalila mthupi,ine ningadalile kupitililapo. ⁵ Ninadulidwa pasiku eiti,pa banthu ba israeli,kubanja ya Benjamini,Mhebeli wa ahebeli,kulingana nalamulo Mfalisi. ⁶ Mwachilakolako ninanzunza mpingo,nili pansi palamulo,ninalibe kadontho. ⁷ Koma zinali zaphindu kwaine,ninazona zilibe phindu kamba ka Yesu. ⁸ Koma manje niwona kuti vinthu vonse vilibe phindu,chifukwa kuziba Yesu ChristuK kwa koyendelela.Kamba ka eve ninataya vonse.Niviona vilibe phindu kuti nikaphindule mwa Yesu, ⁹ Nakupezeka mwa eve.Nilibe chiyelo changa neka kuchokela ku lamulo.Koma nili nachiyelo chopyoleda mu chikhulupililo mwa Yesu,Chiyelo chochokela kwa Mulungu kupyolela mu chikhululupililo. ¹⁰ Apa nimufuna nimuzibe na mphamvu ya kuukisiwa kwake,nachiyanjano manzunzo yake.Nifuna kusinthisiwa muchifanizilo cha imfa yake. ¹¹ Kuti mwina ninga mnvesese phamvu yakuukisidwa kuchokela ku infa. ¹² Sivazooni kuti nalandila kudala ivi vinthu,kapena kuti nasiliza.koma nipushinga kuti nikalandile chamene Yesu Christu ananikonzele. ¹³ Abale siniganiza kuti nalandila kale.Koma pali chinthu chimozi chamene nichita.Niibalako vakumbuyo nayanganila vakusogolo, ¹⁴ Nithamanga nilikuyanga pothela yawilo,kuti nikawine mphoto yamaitanidwe ¹⁵ Tonse ise tilibakulu,tiyeni tiganize munjila iyi,elo ngati muganiza mosiyana pachilichonse,Mulungu azavumbulusa icho kwa imwe. ¹⁶ Koma pamene tafika tiyeni tigwilisise. ¹⁷ Nkhalani okopelela ine abale.Muziyanganila kulibamene bayenda mwachisanzo chamene chilimuli ise. ¹⁸ Bambili bayenda,baja bamene ninamuuzaniponi,elo manje nimuzani namisozi,monga adani ba mtanda wa Yesu. ¹⁹ Chifukwa sogolo yao nichionongeko.chifukwa mulungu wao ni mimba zao,kuzitukumula kwao kuli mumanyazi yao.Baganiza pa zinthu zapaziko. ²⁰ Koma ise kwathu nikumwamba,kwamene tiyembekeza mupulumusi,mbuye Yesu christu. ²¹ Azasintha mathupi yathu kunkala mathupi monga yake yamuulemelo,yopangiwa na phamvu yake,kuti vonse vikagonjele iye.

Chapter 4

¹ Motero abale banga bamene nifunisisa kuona, pakuti chimwemwe na kolona yanga, munjila iyi imililani mwambuye. Okondedwa banga. ² Nipapatila Euodia, nipapatila futi Syntyche, nkhalani na nzelu zimozi mwa Yesu. ³ Inde nimupapatilani naimwe, mnzanga mugoli imozi. Thandizani aba azimai. Chifukwa banasebenza naine mukulalikila uthenga na Clement na awo onse anchitho anzanga, amene mazina yao yali mu buku ya moyo. ⁴ Sangalalani mwa Ambuye nthawi zonse. Nafuti nikamba kuti sangalalani. ⁵ Lekani kufasa kwanu kuzibike kwa muthu aliyense. Abuye alipafupi. ⁶ Musade nkhwapa pachilichonse, koma muzonse na pempelo nazofuna zanu, namayamiko, lekani zofuna zanu zizibike kwa Mulungu. ⁷ Ndipo mtendere wa Mulungu, wamene upitilila mamvesedwe yonse, uzachingiliza mitima na maganizo yanu mwa Yesu Christu. ⁸ Posilizila, abale, vilivone bazooni, vilivonse vaulemu, vilivonse vabwino, vilivonse voyera, vilivonse vokondewa, chilichonse chauthenga uthenga wabwino, ngati pali chilichonse chopambana, ngati pali chilichonse choyenera matamando, muganize pali ⁹ ivi. Vinthu vamene mwamene mwaphunzila nakulandila, nakumvela, navamene mwaona muli ine, chitani ivi, ndipo mulungu wa mtendere azankhala naimwe. ¹⁰ Nimasangalala maningi mwa Ambuye chifukwa manje pothela mwankala muniikako nzelu. Munali kuniikakao nzelu kudala, koma mwenzelibe danga yonithandiza. ¹¹ Sinikamba ichi kamba kakuti nineosobeka. Pakuti ninaphunzila kunkhala okhutila munthawi zonse. ¹² Niziba kunkhala osauka nakunkhala na vambili. Munjila iliyonse namuvonse, nazindikila chinsinsi chodyesewa bwino kapena kunkhala na njala, kunkhala na vambili nakhala osoba. ¹³ Ningachite vonse vinthu kupyolela mwa eve wamene anipasa mphamvu ine. ¹⁴ Koma munachita bwino kugabana naine muzobvuta zamene ninpitamo. ¹⁵ Imwe Afilipi muziba kuti pachiyambi cha uthenga, pamene ninachoka ku macedonia kuti, palibe mpingo unanithandiza muzakupasa kapena kulandila koma imwe chabe. ¹⁶ Nangu pamene nenzeli ku tesalonica munanitumizila thandizo kupitilila kamozi. ¹⁷ Sikuti nifuna mphaso koma chipaso chamene chichokela mukupeleka kwanu. ¹⁸ Nalandila vinthu vonse, ndipo ninavambili. Nankhala okhutisidwa. Nalandila vinthu vamene munanitumizila kuli Epaphroditus. Nivinthu vabwino vonunkhila, nsembe yokondwelesa kwa Mulungu. ¹⁹ Mulungu wanga azmupasani zofuna zanu zonse kulingana na kulemela kwake muulemelo mwa Christu Yesu. ²⁰ Manje kuli Mulungu Atate bathu kunkhale ulemelelo wamuyayaya. Amen. ²¹ Mupase moni okhulupilila aliyense mwa Yesu Christu. ²² Abale balinaine bakupasani moni kuno, makamaka bamene bali munyumba ya Kaesala. ²³ Chisomo cha ambuye Yesu Christu chinkhale na Muzimu wanu.

Colossians

Chapter 1

¹ Paulo, mtumwi wa Kristu Yesu kupitila mucifunilo ca Mulungu, na Timoteyo mubale wathu, ² kuli okhulupilila na okhulupililika abale mwa Kristu amene ali ku Kolose. Lekani cisomo cikhale kwa imwe, na mtendele kucokela kuli Mulungu Atate bathu ndi Ambuye Yesu Kristu. ³ Tipeleka mayamiko kwa Mulungu, Atate bake ba Ambuye bathu Yesu Kristu, ndipo tikupemphelelani nthawi zonse. ⁴ Tinamvela za cikhulupiliro canu mwa Kristu Yesu na cikondi camene muli naco pa onse anapatuliwila Mulungu. ⁵ Muli na cikondi ici cifukwa ca ciyembekezo cikhulupililika cinasungiwila imwe kumwamba. Munamvelapo za ciyembekezo cikhulupililika mu mau ya zooni, uthenga wabwino, ⁶ wamene unabwela kwa inu. Uthenga wabwino uyu ubala zipaso ndipo ukula muziko lonse. Wankhala ucita ici mwa imwenso kuyambila siku munaumvela nophunzira za cisomo ca Mulungu mu coonadi. ⁷ Uyu ndiye uthenga wabwino wamene munaphunzila kucokela kuli Epafulasi, okondeka wanchito muzathu, wamene aliwanchito okhulupililika wa Kristu mumalo mwathu. ⁸ Epafulasi watizibisa ise za cikondi canu mu Mzimu. ⁹ Cifukwa ca cikondi ici, kuyambila siku yamene tinamvela izi sitinaleke kukupemphelelani imwe. Tankhala tipempha kuti munkhale ozulisiwa pakuzi za cifunilo cake mu nzeru zonse nakumvesesa za uzimu. ¹⁰ Tankhala tipephela kuti muzayenda moyenela mwa Ambuye munjila zokondwelesa. Tankhala tipephela kuti muzalimbikisika muzocita zili zonse kulingana na mphamvu za ulemelelo wake mukupitilila konse na kuleza mtima. ¹² Tipephela kuti mosangalala muzapeleka mayamiko kwa Atate, wamene akupangani kukwanisa kugabana mucolandila ca ukhulupilila mukuunika. ¹³ Anaticosa ku ulamulilo wa mumudima notipeleka ku ufumu wa Mwana wake okodeka. ¹⁴ Mu Mwana wake tili nakuombolewa, kukhulukiwa kwa macimo. ¹⁵ Mwana ndiye cithunzi-thunzi ca Mulungu wamene sitiona. Ndiye oyamba kubadwa pa zolengewa zonse. ¹⁶ Kupitila mwa

yeve zinthu zonse zina lengewa, zija zili kumwamba nazija zili pansi, zamene tiona nazamene sitiona. Yangakhale maufumu kapenda ma ukulu olo ma boma kapena ma ulamulilo, zonse zinthu zinalengewa nayeve ndipo kwa yeve.¹⁷ Enzeko kukalibe kunkhala zili zonse, ndipo mwa yeve zinthu zonse zikwilizana pamozi.¹⁸ Ndipo ndiye mutu wa thupi, mupingo. Ndiye oyamba ndipo obadwa oyamba kucolela pakati pa akufa, telo ali namalo oyamba pakati pa zinthu zonse.¹⁹ Mulungu enze okodwela kuti umulungu bonse unkhale mwa yeve,²⁰ ndipo kuti abwelese kwa iye zinthu pamozi kupitila mwa Mwana. Mulungu anayanjanisa zinthu zonse kwa iye, zingankhale zinthu za pansi kapena za kumwamba.²¹ Ndipo naimwenso pa nthawi inangu mwenze acilwendo kwa Mulungu mdipo mwenze adani bake mumaganizo namuzocita.²² Koma manje wakuyanjanisani mu thupi yake kupitila mu imfa. Anacita tele kuti akupelekeni oyela, alibe cifukwa, ndipo osapezeka na milandu kuli yeve,²³ ngati mupitiliza mucikhulupililo, onkhazikika na osagwendezeka, osati ocoka ku ciyembekezo ca cisimikizo ca uthenga wa bwino wamene unalalikiwa kwa munthu aliyense analengewa pa ziko la pansi. Uyu ndiye uthenga wamene ine Paulo ninankhala kapolo.²⁴ Manje nikondwela muzovuta zanga cifukwa ca imwe. Ndipo ninkhala nazo muthupi mwanga zamene zili zosoba zobaba za Kristu cifukwa ca thupi yake, wamene uli mpingo.²⁵ Nificukwa ca mpingo uyu wamene ine nili kapolo, kulingana nanchito yocokela kwa Mulungu camene cinapasiwa kwa ine cifukwa ca imwe, kukwanilisa mau ya Mulungu.²⁶ Ici ndiye cinsinsi ca zooni camene cinabisiwa kwa nthawi itali ndipo kwa mibado. Koma manje canazibisiwa kuli baja bamene anakhulupilila mwa iye.²⁷ Nikuli beve kwamene Mulungu anafuna kuzibisa kulemela kwa ulemelero kwa cinsinsi ca zooni pakati pa akunja. Ndiye uja Kristu wamene ali mwa imwe, ciyembekezo ca ulemelelo wakusogolo.²⁸ Uyu ndiye wamene tilalikila. Tilimbikisa munthu aliyense, ndipo tiphunzisa munthu aliyense na nzeli zonse, kuti tingapeleke munthu ofikapo mwa Kristu.²⁹ Cifukwa ca ici nisebeza ndipo niyeseza kulinga na mphamvu zamene zisebeza mwa ine mwa mphamvu.

Chapter 2

¹ Nifuna kuti muzibe kubvutika kukulu kwamene nenzelinako pali imwe, kuli baja bali ku Laodisiya, nakuli bambili bamene sanaonepo pamenso panga. ² Sinebenza kuti mitima yabo inkhale yolimbikisiwa pakuletewa pamozi mwa cikondi nazopezeka zolemelesa za cisimikizo comvesesa, namunzeru za cinsinsi cazoona ca Mulungu, ndiye, Kristu. ³ Mwayeve chuma conse ca nzeru nakuziba zinabisika. ⁴ Nikamba so kuti kulibe wamene azakunamizani boza namau yacinyengo. ⁵ Ndipo ngankhale sinilinna imwe mu thupi, koma nili na imwe mu mzimu. Nisangalala poona ndondomeko zanu za bwino nakulimbikila kwa cikhulupililo canu mwa Kristu. ⁶ Monga mwamwene munamulandilila Kristu Ambuye, yendani mwa iye. ⁷ Nkhalani oshikika mwa yeve, omangiwa pa yeve, okhazikika mu cikhulupililo, monga mwamene muphunzisiwila, ndipo osefukila mu mayamiko. ⁸ Onani kuti kulibe amene akumangani kupitila muphunzilo ya umunthu namanganizo ya boza kulingana na mwambo wa banthu, kuzipeleka ku zinthu zamaphunziso ya ziko, ndipo osati kuzipeleka kwa Kristu. ⁹ Cifukwa mwa iye munkhala umunthu wa Umulungu bonse. ¹⁰ Ndipo ndimwe ozulisiwa mwa iye. Ndiye olamulila mphamvu nama ulamulilo bonse. ¹¹ Mwa yeve munacitiwanso mudulidwe, namudulidwe osacitika na banthu pakucosa thupi ya munyofu, koma mumudulidwe wa Kristu. ¹² Munafakiwa naye mumanda kupitila mu ubatizo. Ndipo mwa yeve munaukisiwa kupitila mucikhulupililo mu mphamvu ya Mulungu, wamene anamuukisa kwa akufa. ¹³ Ndipo pamene munali akufa mu macimo yanu ndipo namukusadulidwa kwa thupi yanu, anakupangani amoyo pamozi nayeve notikhululukila tonse macimo yathu. ¹⁴ Anafafaniza mbiri yolembewa ya nkhangole namalamulo yosushana na ife. Anaicosa yonse ndipo anakhomalela pa mtanda. ¹⁵ Anagonjesa mphamvu na maulamulilo, ndipo anazionesa kubanthu, pakunkhala opambana kupitila mu ntanda. ¹⁶ Cifukwa ca ici pasankale munthu wamene azakuweluzani pazakudya kapena pa zakumwa, kapena kukamba siku yosangalala kapena siku ya mwezi wasopano, kapena pa siku la Sabata. ¹⁷ Izi nizithunzi-thunzi za zinthu zamene zizabwela, koma cinthu cene cene ni Kristu. ¹⁸ Pasankhale munthu wamene afuna kuzicepesa nakupembeza angelo akuweluzeni pakukucosani pa mphoto yanu. Uyu munthu alowa muzinthu zamene anaona ndipo amabwela azitukumula cifukwa camanganizo ya umunthu. ¹⁹ Sagwililila kwa Yesu amene ali mutu. Nikocokela kumutu kwamene thupi yonse kupitila mumajoini na mizipe zilandila nogwililana pamozi, cikulila pamozi nakukula kwamene Mulungu apasa. ²⁰ Ngati munafa pamozi na Kristu kuzithu zakuno kucalo, nicifukwa nicani munkhala ngati muli pansi pa ulamulilo wa calo: ²¹ "Musagwile, musalabe, musacikumye"? ²² Izi zonse zizaonengeka pamene zisebenzesewa, kulingana namalangizo na ziphunziso za banthu. ²³ Aya malamulo yali nanzelu zacipembezo co pangiwa na munthu mwine wake nakuzicepesa nakusadalila thupi. Koma zilibe mphindu pazocita zomvesa bwino za thupi.

Chapter 3

¹ Manje ngati Mulungu akukwezekani pamozi na Yesu, sakilani zinthu za kumwamba, kwamene Kristu ankhala pa kwanja ya manja ya Mulungu. ² Ganizilani zinthu za kumwamba, osati zinthu za pansi. ³ Cifukwa imwe munafa, ndipo moyo wanu niwobisika na Yesu mwa Mulungu. ⁴ Pamene Yesu azaonekela, wamene ali moyo wanu, ndiye kuti naimwe mu zaonekela pamozi na yeve mu ulemelelo. ⁵ Cifukwa ca ici, payani zinthu zamene zili za ziko -ciwelewele, cofipisa, kufuna zoipa, cilako lako coipa, naku khubwila, camene cili kupembeza ma mafano. ⁶ Nicifukwa ca izi zinthu camene mukwiyo wa Mulungu uzabwela pa bana osamvera. ⁷ Nimuzinthu monga izi zamene imwe nunayendamonso kudala pamene mwendo nkhalamo. ⁸ Koma manje mufunika kutaya zinthu zonse izi -mukwiyo, kukalipa, manganizo oyipa, manyozo, kukamba zonyansa kucoka mu kamwa mwanu. ⁹ Musanamizane wina na muzace, cifukwa munacosa munthu wakudala uja nazocita zake, ¹⁰ ndipo mwabvala munthu wasopano wamene apangiwa wasopano mukuziba kulingana nacifanizo cawamene anamupanga. ¹¹ Apa ndiye cifukwa cake kulibe mu Giriki namu Yuda, odulidwa kapena osadulidwa, wakunja, ocimwa, kapolo, waufulu koma Kristu ndiye zonse, ndipo ali muli zonse. ¹² Bvalani, manje, monga osankiwa ba Mulungu, oyela na okondewa, mtima wacifundo, abwino mtima, ozicepesa, osabilima, oleza mtima. ¹³ Mvesesanani wina na muzake. Nkhalani acisomo kuli wina namuzake. Ngati winangu ali na dandaulo pali muzake, khulukililanani monga Ambuye anaku khulukililani. ¹⁴ Pamwamba pa zonse izi, nkhalani na cikondi, camene cimangilila zonse bwino. ¹⁵ Lekani mtendele wa Kristu ulamulile mumitima yanu. Nicifukwa ca mtendele uyu kuti munaitaniwa mu thupi imozi. Ndipo nkhalani aciyamiko. ¹⁶ Lekani mau ya Kristu yankhale yambili mwa imwe. Na nzeru zonse phunzisani nolimbikisana wina na mzake kupitila mu masalimo na nyimbo na nyimbo za uzimu. Imbani na ciyamiko mu mtima mwanu kwa Mulungu. ¹⁷ Ndipo zonse mucita, mu mau, kapena muzocita, citani zonse mu zina ya Ambuye Yesu. Pelekani ciyamiko kwa Mulungu Atate kupitila mwa iye. ¹⁸ Akazi, mvelelani ba muna banu, monga cili coyenela mwa Ambuye. ¹⁹ Amuna, kondani ba kazi banu, ndipo musankhale obakwiwila beve. ²⁰ Bana, mvelelani makolo banu muzinthu zonse, cifukwa ici nicokondwelesa mwa Ambuye. ²¹ Azitate, musakalipise bana banu, kuti basabwezewe pansi. ²² Akapolo, mverelani mambwana banu muzinthu zonse kulinga nazakuthupi, osati kusebenza kuti bakuoneni kapena kukodwelesa banthu, koma na mtima wa zoona. Yopani Ambuye. ²³ Cili conse camene mucita sebezani kucoka pansi pa mtima monga musebenzela Ambuye osati banthu. ²⁴ Muziba kuti muzalandila mphoto yacolowa kucokela kwa Ambuye. Ndi Ambuye Kristu wamene mutumikila. ²⁵ Aliyense wamene acita cosalungama azalandila cilango pa vosalungama vamene acita, ndipo kulibe kukondela.

Chapter 4

¹ Mabwana, pasani akapolo zoyenela na zamuyeso wabwino. Muziba kuti muli nabwana namwenso kumwamba. ² Pitilizani mokhulupililika mu maphemphelo. Nkhalani chelu mwamene umo muciyamiko. ³ Mutipemphelere pamozi ise, kuti Mulungu angasengule ciseko camau, kuti tikambe cinsinsi ca zooni ca Kristu. Cifukwa ca ici, ndine omangiwa. ⁴ Ndipo pemherani kuti ndicionese bwino, monga niyenela kukamba. ⁵ Yendani mwa nzeru kuli akunja, ndipo musebenzese bwino nthawi. ⁶ Lekani mau yanu nthawi zonse yankhale na cisomo. Lekani yankhale yomveka bwino, kuti mungazibe mwamene mungayankhele munthu aliyense. ⁷ Pazinthu zokhuzana naine, Taikikasi azakuzibisani imwe. Nimubale okondeka, wanchito wokhulupililika, kapolo muzathu mwa Ambuye. ⁸ Ninamutumu kwa imwe cifukwa ca ici, kuti mungazibe zokhuzana na ise ndipo kuti alimbikise mitima yanu. ⁹ Ninamutuma pamozi na Onisimasi, mubale okhulupililika na okondeka, wamene ali umozi wa imwe. Azakuuzani zonse zacitika kuno. ¹⁰ Aristakasi, wandende muzanga akupasani moni, cimozi mozi na Mariko khazeni wa Banabasi (wamene mwenze munalandila malamulo yakuti; ngati azabwela kwa imwe, mumulandile), ¹¹ ndipo nayenve Yesu wamene ayitaniwa kuti Jasitasi. Aba beve amudulidwe nibanchito banzanga mu ufumu wa Mulungu. Akhala onitonthona ine. ¹² Epafulasi akupasani moni. niumozi wa imwe ndipo kapolo wa Kristu Yesu. Nthawi zonse alimbikila kupemphela imwe, kuti muimilile mofikapo nacisimikizo cokwanila mucifunilo conse ca Mulungu. ¹³ Nipelekela umboni pa iye, kuti asebenza mwa mphamvu cifukwa ca imwe, kuli baja bali ku Laodikiya, nabaja ali ku Hirapolis. ¹⁴ Luka dotolo okondeka na Demasi akupasani moni. ¹⁵ Mubapase moni abale amene ali ku Laodisiya na Nimpha, namupingo wamene uli munyumba mwake. ¹⁶ Pamene kalata iyi izabelengewa pakati panu, mukaibelenge futi mu mpingo wa banthu aku Laodisiya, ndipo muone kuti muberenganso kalata yocokela ku Laodisiya. ¹⁷ Mukambe kuti kwa Achipasi, "Yangana ku utumiki wamene unalandila mwa Ambuye, kuti ubukwanilise." ¹⁸ Uyu moni nalemba na kwanja kwanga -Paulo. Kumbukilani kumangiwa kwanga. Lekani cisomo cinkale na imwe.

1 Thessalonians

Chapter 1

¹ Paulo, Silvano, na Timoteyo ku mpingo wa ku Tesalonika mwa Mulungu Atate na Ambuye Yesu Kristu. Chisomo na mtendere unkale na imwe. ² Timayamikila Mulungu nthawi zonse chifukwa cha imwe, pamene tikamba za imwe muma pemphero yatu. ³ Tikumbukila mosalekezela pamaso pa Mulungu nchito zanu za chikulupiliro, nchito za chikondi, na kuleza mutima koma futi chisimikizo cha msogolo mwa ambuye wathu yesu khristu. ⁴ Abale okondedwa ni ambuye, tiziba bakusankhani inu, ⁵ Chifukwa cha uthenga wa mulungu unaza kwa inu osati mu mau chabe komanso mu mphamvu, ya Muzimu Oyera, na chisimikizo cha mphamvu. chimozi-mozi, muziba tinali banthu ba bwanji pakati panu chifukwa cha inu. ⁶ munankhala olondola bathu komanso ba ambuye, pamene munalandira mau mumabvuto yambiri mokondwa kuchoka kwa muzimu oyera. ⁷ Mwa ichi, munankhala chisanzo kwa onse ku macedonia ni achaia bamene banakulupilira. ⁸ Chifukwa kwa inu mau ya ambuye yamveka, osati ku macedonia ni achaia. mumalo mwake, kumalo yaliyonse chikulupiliro chanu mwa mulungu chasila. mwa ichi, sitifunika kukamba kalikonse. ⁹ chifukwa beve beka bakamba kuti tinali banthu ba bwanji pamene tinali kubwera pakati panu. bakamba mwamene munabwera kwa mulungu kuchoka ku mafano kutumikila mulungu wa moyo na wa zooni. bakamba kuti ¹⁰ muyembekeza mwana wake kuchoka ku mwamba, wamene anamuukisa kwa akufa. uyu ni hyesu, wamene atitabisa ku zowawa zamene zizabwera.

Chapter 2

¹ Inu mweka muziba, abale, kuti kubwera kwathu kwa inu sikunali kopanda nchito. ² Muziba kuti tinabvutika poyamba komanso tinachitidwa manyazi ku afilipi. tinali olimba mwa mulungu wathu kulankhula nanu za mau ya mulungu mobvutikila. ³ Chifukwa kuyamikidwa kwathu sikunali kwangozi, kapena kwa kudesedwa, kapena kwa chinyengo. ⁴ Mumalo mwake, monga mwamene mulungu watiyeneleza kuti tikhale okulupilika mu mau ya mulungu, kuti tikambe. tikamba, osati kuti tikondwerese banthu, koma kuti tikondwerese mulungu. niwamene amaona mitima yathu. ⁵ Sitimagwiritsa nchito mau yoipa pa nthawi ina iliyonse, monga muziba, kapena kamba ka kukumbwila. chifukwa mulungu ndiye mboni yathu. ⁶ Kapena tinapempha ulemelero kuchoka ku banthu, kwa inu kapena benangu. tinakafuna ukondeledwa monga atumwi ba khristu. ⁷ Mumalo mwake, tinali odekha mtima pakati panu monga muzimai atonhoza ana ake. ⁸ Mu njira iyi tinali na chikondi na inu. tinali okondwa kugawana na inu osati thenga chabe wa mulungu komanso miyoyo yathu. chifukwa munankhala okondwedwa kwambiri kwa ife. ⁹ Pakuti mukumbukira, abale, nchito yathu na kubvutika kwathu. usana na usiku tinali kugwira nchito kuti tisamibwezeni kumbuyo. pa nthawi ija, tinalalikira kwa inu uthenga wa mulungu. ¹⁰ Ndimwe mboni, na mulungu, mwamene mulili oyera, opanda chilema, komanso oliungama tinankhala bwino kwa inu okulupilika. ¹¹ Mu njira imozi-mozi muziba mwamene tinankhalira na wina aliyense monga atate achitira na bana bake, tinali kukupapatirani na ¹² Kukulimbikisani na kukupemphani kuti muyende munjira yoyenera pamenso pa mulungu, wamene anamuitanani mu ufumu wake. ¹³ Mwa ichi tiyamika mulungu mosalekeza. chifukwa pamene munatilandira uthenga wa mulungu wamene munamvera kuchoka kwa ise, munayalandira osati monga mau ya munthu. mumalo mwake, munayandila mwamene yalili, mau ya mulungu. ni mau yamene aya yamene yagwira nchito pakati panu okulupilira. ¹⁴ Kwa inu, abale, munankhala okonkha ba mipingo ya mulungu yamene yali ku yudeya mwa khristu yesu. chifukwa naimwe munabvutika zinthu zimozi kuchoka ku anthu bamozi-mozi, mwamene banachitira bayuda. ¹⁵ Ni bayuda bamene banapaya ambuye yesu na baneneri. ni bayuda bamene banatipisha. sibakondweresa mulungu. mumalo mwake, bali na nkhanza ku banthu bonse. ¹⁶ Batilesa kukamba na bamitundu kuti bapulumuke. chosatira ni chakuti bapakisa machimo yao. chilango chiyenera kufika pa iwo pothera. ¹⁷ Ndise opatulidwa kwa inu, abale, kwa ka nthawi kang'ono, muthupi osati mu mutima. ndise okonzeka, na kufunisisa, kuona nkhope yanu. ¹⁸ Chifukwa tinafunisisa kubwera kwa inu, ine , paulo, nafuti, koma satana anatilesa. ¹⁹ Chiyembekezo chathu cha kusogolo ni cha bwanji, kapena chimwemwe, kapena kolona yotikondweresa pamenso pa ambuye yesu pa kubwera kwake? si inu na benangu? ²⁰ Chifukwa ndimwe chimwemwe na ulemelero wathu.

Chapter 3

¹ Koteru, pamene sitinakwanise kuchisunga, tinaona chinali bwino kutisiya ku athens teka. ² Tinatuma timoteyo, m'bale wathu na ogwira naye nchito mwa mulungu mu uthenga wa khristu, kuti akulimbiseni nakuku tonthozani mu chikhulupiliro. ³ Tinachita izi kuti winangu asagwedezeke na mabvuto awa. chifukwa inu muziba kuti pa ichi tinasankhidwa. ⁴ Zoonadi, pamene tinali na inu, tinakuuzani poyamba kuti tinali kufunika kubvutika, ndipo izi zinachitika, monga muziba. ⁵ Mwa ichi, pamene sininakwanise kuimilira, ninatuma kuti nizibe za chikulupiliro chanu. mwina oyesa uja anakuyesani mu njira ina yake, na nchito yathu inali yopanda phindu. ⁶ Koma timoteyo anabwera kuchoka kwa inu na kuleta kwa ise uthenga wabwino wa chikulupiliro na chikondi. anatiuza kuti mumatikumbukira, na kuti mufuna kutionanso monga mwamene ise tifunila kukuonani. ⁷ chifukwa cha ichi, abale, tinatonthozedwa chifukwa cha chikulupiliro chanu, mumabvuto yathu yonse na kunzunzidwa. ⁸ tsopano tili na moyo, ngati muimilira mwa ambuye. ⁹ nimatokozo ya bwanji yamene tingapase mulungu pa inu, pa chimwemwe chonse chamene tili nacho pamenso pa mulungu cha inu? ¹⁰ usiku na muzuba timakupemphelerani na mphamvu kuti tione nkhope yanu na kukupasani chamene chipelebera pa chikulupiliro chanu. ¹¹ lekani mulungu atate athu yeve, na ambuye yesu, atipase njira yofika kwa inu. ¹² mulungu akupangiseni kuti mukule mu chikondi cha wina na mnzake na banthu bonse, mwamene naise tichitira kwa inu. ¹³ alimbise mitima yanu, kuti yankhale yopanda zodesa mu chiyelo pa menso pa mulungu atate, pa kubwera kwa ambuye yesu na bonse boyera.

Chapter 4

¹ Mosiliza, abale, tikulimbikisani and kukukoselesani mwa Ambuye Yesu Kristu. Monga mwamene munalandilira ma lamulo kuchokela kuli ise mwamene muyenela kuyendela na kumvesa bwino Mulungu, mwamene umu munjila endani, mwakuti muchite ichi nakuchilapo. ² Chifukwa imwe muziba ma lamulo yamene tinakupasani kupitila muli Ambuye Yesu. ³ Ichi ndiye chifunilo cha Mulungu, kusukiwa kwanu, kuti musiye uchiwere-were, ⁴ kuti aliyense mwa imwe azibe mosungila tupi yake mu chiyelo na mu ulemelelo, ⁵ osati mokonda zilakolako. (monga mwamene amukunja bamene sibaziba Mulungu). ⁶ Osavomeleza muntu ali onse kulakwila na kuchitila choipa mubale wake muli ichi chintu. Chifukwa Ambuye ndiye bamabwezela muvintu ivi, monga mwamene tinaku chenjezelani naku peleka umboni. ⁷ Chifukwa Mulungu sana ti-itanile ku uchimo, koma ku chiyelo. ⁸ Mwa ichi, eve wamene akana ivi sakana bantu, koma Mulungu, wamene apeleka Muzimu Oyela kuli imwe. ⁹ Kulangana pa chikondi cha ubale, imwe simuyenekela kuti muntu amulembeleni pa ichi, chifukwa imwe muma punzisiwa na Mulungu kuti mukondane wina na muzake. ¹⁰ Zo-ona, mumachita ichi kuli bonse babale bali ku Macedoniya. Koma tikulimbikisani, abale, kuti muchite ichi naku chilapo. ¹¹ Tikulimbikisani futi kuti mufunisise kunkala umoyo ulibe chongo, kuzisamalila ntchito zanu, naku zisebenzela na manja yanu, monga mwamene tinaku uzilani, ¹² mwakuti muyende moyenela pamenso pa bakunja komanso kuti musankale bopelebele. ¹³ Sitizafuna kuti munkale osaziba, abale, pali baja bantu banagona, mwakuti musalile monga bantu bonse, bamene balibe chiyembekezo. ¹⁴ Chifukwa ngati ise tikulupirila kuti Yesu ana mwalila koma anauka nafuti, munjila yamene iyi Mulungu azabaletela pamozi na Yesu bantu bonse banagona mwa eve. ¹⁵ Ichi tikamba kuli imwe mu mau ya Ambuye, kuti ise bamene tikali namoyo, bamene tisalila pa kubwela kwa Ambuye, sitiza chila baja bamene banagona. ¹⁶ Chifukwa Ambuye baza seluka kuchoka kumwamba. Baza bwela naku punda, na liu ya mungeli mukulu, na lipenga ya Mulungu, ndipo bakufa mwa Kristu baza ukisiwa moyamba. ¹⁷ Kukonkapo ise bamene tili na moyo, bamene tinasala kumbuyo, tiza tengewa pamozi mumakumbi kukakuma Ambuye mu mpepo. Munjila yamene iyi tizankala ntawi yosasila na Ambuye. ¹⁸ Mwa ici, tontozani wina na muzake na mau aya.

Chapter 5

¹ Manje kukamba pa zantawi na nyengo, abale, sichofunikila kuti chintu chilichonse chilembewe kuli imwe. ² Chifukwa imwe muziba mofikapo kuti siku ya Ambuye ibwela monga kawalala usiku. ³ Pamene bazakamba kuti, "Mutendere na kuchingiliziwa," koma kuonongeka kosayembekezela kuzabafikila. Chizankala monga kubaba mumimba kwa muzimai ali na pakati. Sibazakwanisa kutaba. ⁴ Koma imwe, abale, simuli mumudima mwakuti ija siku ikakufikileni monga kawalala. ⁵ Chifukwa imwe ndimwe bana ba ku-unika komanso bana bamuzuba. Sindise bana ba usiku kapena mufinzi. ⁶ Mwa ici, tisazivomeleze kugona monga bonse mwamene bagonela. Koma, tiyeni tinkale bolanga komanso bosakolewa. ⁷ Chifukwa baja bamene bagona bagona usiku, nabaja bamene bakolewa bakolewa usiku. ⁸ Koma cifukwa ndise ba mbali ya muzuba, tiyenela kunkala bosalezela komanso kuvala chikululupiro na chikondi monga chochingiliza pa chifuba, ndiponso chiyembekezo cha chipulumuso kunkala chisote. ⁹ Chifukwa Mulungu sanati nkazikisile ukali, koma kutenga chipulumuso kupitila muli Ambuye Yesu Kristu. ¹⁰ Eve niwamene anatifela mwakuti, tiligone kapena tili bo uka, tinkale Naye pamozi. ¹¹ Mwa ichi limbikisanani wina na mzake na kuzi kulisa, monga mwamene muchitila kudala. ¹² Tikupempani, abale, kuti mubazindikile baja bamene basebenza pakati kanu nabaja bamene boyanganila mwa Ambuye naku kukulimbikisani pakati kanu. ¹³ Nafuti tikupempani kuti mubapase ulemu maningi muchikondi chifukwa cha ntchito yabo. Nkalani mumutendere pakati panu. ¹⁴ Tikulimbikisani, abale: chenjelesani baja bamusokonezo, limbikisani bofoka, tandizani balibe mpavu, komanso nkalani bozileza kuli bonse. ¹⁵ Onesesani kuti palibe wamene alipila choipa na choipa kuli muntu ali onse. Koma, konkani chamene chabwino ku muntu ali onse komanso na bantu bonse. ¹⁶ Nkalani bosangalala ntawi zonse. ¹⁷ Pempelani kosaleka. ¹⁸ Mu zonse pelekanani mayamiko. Chifukwa ichi ndiye chifunilo cha Mulungu mwa Yesu Kristu pali imwe. ¹⁹ Osazimya Muzimu. ²⁰ Musasule uneneli. ²¹ Yesani vintu vonse. Gwilililani vamene nivabwino. ²² Chokanikoni ku vonse voipa. ²³ Lekani Mulungu wamutendere akulengeseni kunkala boyela mofikapo. Lekani muzimu wanu onse, moyo, na thupi visungiwe kulibe cholakwa paku bwela kwa Ambuye Yesu Kristu. ²⁴ Wamene akuitanani ni-okululupilika, wamene azakwanisa ichi chintu. ²⁵ Abale, mukazitipempelelako ise. ²⁶ Pasani moni abale bonse na mpyompyono oyela. ²⁷ Niku uzani kupitila mwa Ambuye kuti kalata iyi ibelengeke ku ba bale bonse. ²⁸ Chisomo cha Ambuye Yesu Kristu chinkale na imwe.

2 Thessalonians

Chapter 1

¹ Paulo, Siluvano na Timoti, ku mpingo wa Atesalonika mwa Mulungu ba Tate batu na Ambuye Yesu Kristu. ² Chisomo na mutendere kuli iwe kuchokela kuli Mulungu ba Tate batu na Ambuye Yesu Kristu. ³ Tiyenela kupeleka mayamiko kuli Mulungu chifukwa cha imwe, abale, chifukwa chikulupililo chanu chikula maningi maningi, na chikondi chamene ali onse mwa imwe ali nacho pali wina na muzake. ⁴ Chifukwa chake ise tikamba momvela bwino pali imwe mu mipingo zonse za Mulungu chifukwa cha kupilila kwanu na chikulupililo mu kuvutika kwanu konse, na mu kuvutika kwamene mupitamo. ⁵ Ichi ndiye cho onesa kuweluzi kwa chilungamo kwa Mulungu, mwakuti imwe muka tengeko mbali moyenela mu ufumu wa Mulungu, wamene imwe muvutikila. ⁶ Chifukwa zooni, nicholungama kuti Mulungu abwezele mavuto ku baja bamene bakuvutisani imwe, ⁷ na ku tontoza baja bamene bavutikila pamozi na ise, pamene Ambuye Yesu Kristu bazaonekeselewa kuchokela kumwamba pamozi na bangelo bake bampavu ⁸ mu moto oyaka, kubwezela voipa pali baja bamene sibaziba Mulungu napali baja bamene sibamvela mau ya utenga wabwino wa Ambuye Yesu. ⁹ Bazalangiwa na chionongeko chamuyayaya kuchokapo pa menso pa Ambuye na ulemelelo wa mpavu zao. ¹⁰ Bazachita ichi pamene bazabwela kuza lemekezeka mu bantu babo boyela naku lemekezeka kuli baja bokulupilila, chifukwa umboni watu kuli imwe unakululupiliwa. ¹¹ Chifukwa cha ichi naise tipempela imwe mosasiya, kuti Mulungu watu akuganizileni kunkala boyenela kuitaniwa kwanu pamozi na mpavu zao bakwanilise yonse maganizo yabwino na ntchito yonse ya chikululupilo. ¹² Tipempela kuti zina ya Ambuye watu Yesu ilemekezewe mwa imwe, na imwe mwa beve, kulingana na chisomo cha Mulungu na Ambuye Yesu Kristu.

Chapter 2

¹ Manje kukamba pa kubwela kwa Ambuye watu Yesu Kristu na kunkala pamozi nabo, tikupempani abale, ² kuti musasokonezeke kapena kuvutika mutima, na muzimu kapena na utenga, kapena na kalata yamene ioneka munga yachokela kuli ise, kuneka kuit siku ya Ambuye inabwela kudala. ³ Musaleke wina ali onse kuti akunameni boza. Chifukwa siizabwela mpaka chabe kutaika kwa bena kukachitike, na uja muntu wamene alibe lamulo akaonekele, mwana wa chionongeko. ⁴ Uyu ndiye wamene ashusha na kuzikwezeka pamwamba moshusha wamene aitaniwa kuti Mulungu kapena wamene apembezewa. Chifukwa chake, azankala mu nyumba ya Mulungu na kuzionesa kuti eve ndiye Mulungu. ⁵ Nanga simukumbikila kuti pamene ine ninali na imwe ninakuuzani ivi vintu? ⁶ Manje muziba wamene amulesa, kuti akaonekele pa ntawi yake yabwino. ⁷ Kusebenza kwa uja alibe lamulo kunayamba kusebenza kudala, koma kuli wamene amulesa apa mpaka aka chosewepo poyamba. ⁸ Kukonkapo eve awamene alibe lamulo azaonekela, wamene Ambuye Yesu bazapaya na mpepo yaku kamwa kwabo nakumusiya kunkala alibe pindu paku onekela kwabo. ⁹ Kubwela kwa uyu wamene alibe lamulo kuzankala kamba ka kusebenza kwa Satana na mpavu, voonesela, ¹⁰ na vodabwisa vaboza, na voipa va mitundu zosiyanasiyana kwamene kuza nama baja bamene baonongeka, chifukwa banakana kukonda vazoona kuti bapulumusiwe. ¹¹ Chifukwa cha ichi Mulungu abatumila kunamiwa kwa mpavu mwakuti bakulupilile va boza ¹² kuti baka langiwe bamene sibanakulupilile va zoona koma banapezamo kumvela bwino muli vamene vinalibe chilungamo. ¹³ Koma tiyenela kupeleka mayamiko kuli Mulungu chifukwa cha imwe, abale bokondewa na Ambuye, chifukwa Mulungu anakusankani kunkala vipaso voyambilila kupulumusiwa kupitila mu kuyelesewa na Muzimu na kukulupilila mu va zoona. ¹⁴ Anakuitanani kuli ichi kupitila mu utenga wa bwino, kuti munga tenge ulemelelo wa Ambuye Yesu Kristu. ¹⁵ Mwa ichi, abale, imililani molimbikila nafuti mugwililile myambo zamene imwe munapunzisiwa, mu mau kapena mu kalata yatu. ¹⁶ Manje lekani Ambuye watu Yesu Kristu beka na Mulungu ba Tate batu, bamene banatikonda nakutipasa tontozo yosasila na chiyembekezo chabwino kupitila mu chisomo, ¹⁷ baku tontozeni naku kuimilika mu mitima zanu ntchito ili yonse yabwino na mau.

Chapter 3

¹ Manje, abale, tipempeleleni ise, kuti mau ya Ambuye ya endese nakupelekesewa ulemelelo, monga mwamene chilili naimwe, ² na kuti tinga masuliwe ku bantu boipa bamachimo, chifukwa sibonse bamene bali na chikulupililo. ³ Koma Ambuye niokululupilika, bamene bazakulimbikisani naku kuchingilizani kuli eve oipa. ⁴ Tili nacho chikulupililo mwa Ambuye pa imwe, kuti muzachita koma futi muzapitiliza kuchita vintu vamene tikuuzani. ⁵ Lekani Ambuye basogolele mitima zanu mu chikondi cha Mulungu na mukulimbikila mwa Kristu. ⁶ Manje tikuuzani imwe, abale, muzina ya Ambuye Yesu Kristu, kuti musapezeke na mubale ali onse wamene ankala umoyo waulesi na kusafuna kunkala kulingana na mwambo wamene munalandila kuchoka kuli ise. ⁷ Chifukwa imwe muziba kuti nicho enela kuti imwe mukazikonka ise, chifukwa sitinali kunkala chabe pamene tinali pamozi naimwe. ⁸ Sitinali kudya vakudya va muntu ali onse kosalipila, koma tinali kusebenze usiku na muzuba ntchito yovuta kwambili na mumavuto, kuti ise tisankale cholema kuli ali onse. ⁹ Tina chita njila iyi kuti osati chifukwa tinalibe mpavu pali imwe, koma tina chita ivi kuti tinkale chisanzo kuli imwe, kuti imwe mutikonkeleze. ¹⁰ Chifukwa pamene ise tinali pamozi naimwe, tinakuuzani imwe kuti, "Wamene safuna kusebenza asazidya." ¹¹ Chifukwa timvela kuti pali bena pakati panu bamene bachita ulesi, bosazipeleka ku ntchito, koma makamutola nkani. ¹² Manje aba bamankalidwe ya njila iyi tibalamulila na kubalimbikisa mwa Ambuye Yesu Kristu, kuti basebenze kosapanga chongo nakudya vakudya vabo. ¹³ Koma imwe, abale, musaleme na kuchita ntchito zabwino. ¹⁴ Ngati pali wamene samvela mau yatu mukalata iyi, muswateni ndipo musazipezeka pamozi na eve, kuti achite manyazi. ¹⁵ Koma musamutenge monga mudani, koma muzuzuleni monga mubale. ^{16 17 18} Manje lekani Ambuye bamutendele beve bakupaseni mutendele ntawi zonse minjila zonse. Ambuye bankale naimwe monse. Ine, Paulo, nilemba ivi na kwanja yanga, yamene ni choonesela mukalata ili yonse yamene nialemba. Chisomo cha Ambuye Yesu Kristu chinkale naimwe monse. Amen.

1 Timothy

Chapter 1

¹ Paulo, mutumiki wa Kristu Yesu kulingana na lamulo ya Mulungu mupulumusi watu na Kristu Yesu chiyembekezo chatu, ² kuli Timoteo, mwana wa zooni mu chikulupililo: Chisomo, chisoni, na mutendere kuchokela kuli Mulungu Tate na Kristu Yesu Mbuye watu. ³ Monga mwamene ninaku uzila kuti uchite pamene ninali kuima kuyenda ku Masedoniya, nkala ku Aifeso mwakuti unga lamulile bantu benangu kuti basapunzise chipunziso chinangu. ⁴ Kapena kuti basaike nzelu kuli nkani kapena za mibadwe zosasila. Ivi vimalengesa mukangano osasila mwakuti vitandizile lingo ya Mulungu, chamene chinkala kupitila mu chikulupililo. ⁵ Koma lingo ya lamulo ni chikondi chochokela mu mutima woyela, chikumbum'tima chabwino, koma futi kuchokela ku chikulupililo cha bwino. ⁶ Bantu benangu banaleka ivi vintu kumbuyo nakuyenda kukamba vintu vintu nzelu. ⁷ Bamafuna kunkala bapunzisi ba lamulo, koma sibabenzesa vamene bakambapo kapena vamene basimikiza. ⁸ Koma tiziba kuti lamulo niyabwino ngati muntu aisebenzesa bwino. ⁹ Tiziba kuti, lamulo siinapangiwe muntu olungama, koma baja bamene bapwanya lamulo nabaja bamene sibamvela, baja bantu balibe umulungu na bochimwa, nabaja bamene balibe mulungu na bonyozela. Inapangiwiwa baja bamene bamapaya batate na bamayo babo, baja bopaya, ¹⁰ baja ba chiwelewele, baja bamene bagonana bamuna beka-beka, baja bamene bamaba bantu kubapanga bankala bakapolo, baja baboza, baja baumboni waboza, nabaja bonse bamene bashusha vipunziso vabwino. ¹¹ Iyi lamulo ichokela ku uthenga wabwino waulemelelo wa odalisika Mulungu wamene ananikulupilila na uthenga uyu. ¹² Niyamika Klistu Yesu Mbuye watu. Ananilimbikisa, chifukwa ananiona kunkala okululupilika, naku niika mu utumiki. ¹³ Ninali onyozela, osausa, nafuti wa ndeo. Koma ninalandila chisomo chifukwa ninalikuchita ivi mosaziba koma futi mosakulupilila. ¹⁴ Na chisomo cha a Mbuye chinataikila pamozi na chikulupililo na chikondi chamene chili mwa Kristu Yesu. ¹⁵ Uyu uthenga niwokululupilika koma futi oyenela kuvomelezewa, kuti Klistu Yesu anabwela mu ziko kupulumusa bamachimo. Ine ndine oipisisa pali aba bonse. ¹⁶ Koma chifukwa cha ichi ninapasiwa chisomo, kuti kupitila mwa ine, oyambilapo, Klistu Yesu alangize kupilila kukulu. Anachita ichi kunkala chisanzo kubonse baja bamene bazakulupilila mwa iye kufuna moyo osata. ¹⁷ Manje kwa mfumu ya zaka, wamoyo osasila, saoneka, eve Mulungu eka, kunkale ulemu na kulemekezeka ntawi yosasila. Amen. ¹⁸ Ni ika iyi lamulo pa menso pako, Timoti, mwana wanga, kulingana na uneneli wamene unanenewa pali iwe, kuti umenye nkondo yabwino, ¹⁹ kugwililila

chikululupilo na chikumbum'tima chabwino. Kukana ichi, benangu banaononga chikulupililo chabo.²⁰ Aba ndiye bene Himeneyas na Alekizanda, bamene ninapeleka kuli Satana kuti bapunzisiwe kuti basazinyoza.

Chapter 2

¹ Mwaichi, choyamba pa vonse, nipempa kuti mapempo, mapempelo, kuimililako, na mayamiko ya pelekewe pa bantu bonse, ² mafumu na bonse bali mu ulamulilo, mwakuti tinkale myoyo za mutendere zilibe chiwawa mu umulungu na kulemekezewa. ³ Ichi nichabwino na futi chovomelezewa kuli Mulungu Mpulumusi watu. ⁴ Afuna kuti bantu bonse bapulumuke nakubwela kuziwa za chipulumuso. ⁵ Chifukwa kuli chabe Mulungu umozi, futi kuli chabe oimililako umozi kuli Mulungu na muntu, mwamuna Klistu Yesu. ⁶ Anazipeleka kunkala muomboli kuli bonse, ngati umboni wa pa ntawi yoenela. ⁷ Chifukwa cha ichi ine ninaikiwa kunkala mu ulusi na mutumiki-Niku uzani vazoona, sininama boza iyayi-nafuti mupunzisi wa bakunja kwa chikulupililo na va zoona. ⁸ Mwa ichi, nifuna bamuna ku malo yali yonse bakazipempela na kuimya manja yoyela balibe mukwiyo kapena kushushana. ⁹ Chimozi-mozi bakazi baenela kuvala vovala vo enela, vozilemekeza nafuti vozileza, osati bomanga sisi kapena na golide kapena myala ya yapatali kapena voval va mutengo wapa mwamba, ¹⁰ koma kunkala na vamene voyenela baja bazimai bamene balangiza umulungu kupitila mu zinchito zabwino. ¹¹ Mukazi ayenela kupunzila mosapanga chongo nafuti momvela. ¹² Sinivomeleza mukazi kupunzisa kapena kulamulila mwamuna, koma kunkala moyo ulibe chiwawa. ¹³ Chifukwa Adamu analengewa oyamba, kubwela Eva. ¹⁴ Adamu sananamiwe boza, koma mukazi ananamiwa nakubwela kubkala wochimwa. ¹⁵ Koma, azapulumuka kupitila muku bala bana, koma ngati bazapitiliza mu chikulupililo na mu chikondi na mukusukiwa pamozi na nzelu zabwino.

Chapter 3

¹ Uku kukamba niko kululupilika: ngati muntu ali onse afuna kunkala olanganila, afuna ntchito yabwino. ² Mwa ichi eve o onelela sayenela kunkala na kolakwa. Aenela kunkala mwamuna wa mukazi umozi. Ozilesa, wanzelu, ozisamalila bwino, nafuti olandila balendo. Aenela kukwanisa kupunzisa. ³ Safunika kunkala wamoba, osati wandeo, koma, woleza mutima, wamutendere. Saenela kunkala okonda ndalama. ⁴ Aenela kukwanisa kulamulila banja yake bwino, na bana bake baenela kumumvelela na ulemu onse. ⁵ Chifukwa ngati mwamuna sakwanisa kulamulila nyumba yake, azakwanisa bwanji kusalila kachisi ya Mulungu? ⁶ Asankale otembenuka mwasopano, kuti asazule na kuzitukumula na kugwa mu chiweluzo cha mudyelekezi. ⁷ Aenela kunkala na mbili yabwino kuli baja ba kunja, mwakuti asagwele mu manyazi na musampa wa mudyelekezi. ⁸ Ma dikoni, munjila imozo-mozi, bankale bozilemekeza, bachilungamo mukamwa. Basankale ba moba maningi kapena bozikonda. ⁹ Bayenela kusunga chazooni chovumbulusiwa cha chikulupililo na mutima oyela. ¹⁰ Bayenela kunkala bovomelesewa poyamba, pambuyo pake bayenela kutumikilachifukwa balibe cholakwa. ¹¹ Minjila imozo-mozi, bakazi babo bankale bozilemekeza, osati bonyozela, koma banzulu nafuyi bozilemekeza mu vintu vonse. ¹² Ma dikoni bayenela kunkala bazimuna ba mukazi uumozi. Bayenela kukwanilisa bana babo bwino na ma nyumba yabo pamozi. ¹³ Chifukwa baja bamene bana tumikila bwino bazitengela beka zina yabwino na kumvela bwino mu chikulupililo chamene chili mwa Klistu Yesu. ¹⁴ Pamene ine nilemba ivi vintu kuli iwe, nifunisisa kubwela kuli iwe posachedwa apa. ¹⁵ Koma ngati na chedwa, nilemba ivi kuti iwe uzibe mwamene uyenela kuzisungila mu nyumba ya Mulungu, yamene ni kachisi ya Mulungu wa moyo, choimililako na kuimilikisa cha zooni. ¹⁶ Tonse tivomela kuti chisinsi cha umulungu ni chikulu: "Anaonekela mu umuntu, Muzimu Oyela unalangiza kuti anali wa zooni, anaonekela kuli ba ngeli, analalikiwa pa ma iko, anakululupiliwa mu ziko, na kutengewa mu ulemelelo."

Chapter 4

¹ Manje Muzimu ukamba poonekela kuti pa kusila kwa ma siku bantu benangu bazasiya chikulupililo na kuika nzelu ku mizimu ² zaboza na vipunziso va mizimu zonyansa ma boza, mitima zao zinaononge kelatu. ³ Bazayamba kulesa bantu kuti basakwatile nakufuna kuti basazidya vakudya vinangu vamene Mulungu analengela kuti vilandiliwe na mayamiko kuli baja bamene bakulupilila nafuti baziba vazoona. ⁴ Chifukwa vonse volengewa na Mulungu nivabwino. Kulibe chamene tikudya na mayamiko chiyenela kukaniwa. ⁵ Chifukwa china sukiwa na mau ya Mulungu na pempelo. ⁶ Ngati uika ivi pamenso pa ba bale. uzankala kapolo wabwino wa Yesu Klistu. Chifukwa udyesewa na mau ya chikulupililo na vipunziso vabwino vamene iwe unakonka. ⁷ Koma kana nkani za muziko zamene zikondewa na azimai bakulu. Koma, zipunzise mu va umulungu. ⁸ Chifukwa kupunzisa thupi ni kwa pindu ingono, koma umulungu niwa ntchito konse-konse. Ipeleka yanjano mu umoyo uno na mu umoyo wamene ubwela. ⁹ Uyu utenga niwo kulupilika koma futi niwoyenela kuvomelezewa. ¹⁰ Nichifuka cha ichi chamene ise chiyesesa kusebenza maningi. Chifukwa tiyembekezela muli Mulungu wa moyo, wamene ni Mupulumusi wa bantu bonse, maka-maka baja bokulupilila. ¹¹ Lalika na kupunzisa ivi vintu. ¹² Usavomeleze ali onse kusula uchichepele wako. Koma, kuli baja bokulupilila, nkala chisanzo mu ma kambidwe, kankalidwe, chikondi, kunkala okulupililika, na kuyela. ¹³ Mpaka nikabwele, ika nzelu kubelenga, kuchilimbikiso, na kupunzisa. ¹⁴ Usalekelele mpaso yamene ili muli iwe, yamene inapelekewa kuli iwe kupitila mu uneneli, muku ikiwa manja ya ba kulu ba mupingo. ¹⁵ Samalila ivi vintu. Nkala muli vemve, kuti kuyenda pasogolo kwako kuonekele kuli bonse bantu. ¹⁶ Samalila umoyo wako na chipunziso. Pitiliza muli ivi. Chifukwa mu kuchita ivi, uzazi pulumusa weka pamozi nabaja bamene bamvelela iwe.

Chapter 5

¹ Osazuzula muntu mukulu pali iwe. Koma, mulimbikise monga ni tate. Limbikisa bachinyamata monga babale, ² bazimai bakulu monga mai, na basikana monga balongo, muku yela monse. ³ Lemekeza bazimai bofewa, bofewa choona. ⁴ Koma ngati ofedwa ali na bana kapena bazukulu, lekani bayambilile kulangiza ulemu muma nyumba yabo poyamba. Lekani babwezele makolo yabo, chifukwa ichi chimvesa bwino Mulungu. ⁵ Koma uja wamene niofedwa mu cha zoona, wamene anasala eka chabe, aika chiyembekezo chake mwa Mulungu nafuti apitiliza kupeleka ma pempelo naku yapeleka usiku na muzuba. ⁶ Koma, uja muzimai wamene ankala moyo ozimvesa bwino niwakufa kudala ngakale kuti ali na moyo. ⁷ Peleka aya ma lamulo futi, mwakuti bankale balibe kolakwa. ⁸ Koma ngati muntu sakwanisa kusamala ba banja yake, maka-maka baja ba munyumba yake, eve akana chikulupililo futi ali oipa kuchila uja osakulupilila. ⁹ Musaleke muzimai wa zaka zosakwanila sikiste kulembewa kunkala ofewa, mukazi wa mwamuna umozi. ¹⁰ Aenela kunkala ochuka chifukwa cha zinchito zabwino, ichi chingankale kuti analikusamalila bana, kapena anali olandila balendo, kapena anasuka mendo ya bantu boyela ba Mulungu, kapena anatandizila bama vuto, kapena anali ozipeleka ku ntchito zonse zabwino. ¹¹ Koma kubaja bofedwa bango'no, kana kubalemba ma zina. Chifukwa ngati bazipeleka ku zakutupi zoshushana na Klistu, bazafuna kukwatiliwa. ¹² Mukuchita ivi bankala bovutika mitima chifukwa bapwanya pangano yabo yoyamba. ¹³ Pa ntawi imozi, bapunzila kunkala baulesi boyenda kupitana pitana muma nyumba. Sibamankala chabe baulesi, koma bakamba vintu vilibe nzelu nafuti kunkala botaya ntawi, kungo kamba vintu vamene sibayenela kumba. ¹⁴ Ine nifuna kuti bakazi bang'ono bakwatiliwe, bankale na bana, basunge banja yabo, osati kuti bakazipasa mupata kuli mudani kuti akazitinyosa ise. ¹⁵ Chifukwa benangu banakonka kudala Satana. ¹⁶ Ngati mukazi ali onse okulupilila ali na bofedwa, lekani aba tandize, mwakuti kachisi isankale na vochita vambili, kuti itandizile baja bamene nibofedwa mucha zoona. ¹⁷ Lekani ba kulu ba mpingo bamene balamulila bwino baganiziliwe boyenela kulandila ulemu ukulu, maka-maka baja bamene basebenzela mu utenga na muku punzisa. ¹⁸ Chifukwa ma lemba ya kamba kuti, "musa mange ngo'mbe kukamwa pamene ikutwa milisi" koma futi "Eve osebenza aenela malipilo yake." ¹⁹ Osalandile mulandu uli onse pali mukulu wa mupingo koma ngati ngati kuli bakamboni babili kapena batatu. ²⁰ Zuzula bochimwa pasogolo pa bonse kuti bonse bankale na manta. ²¹ Niku pasa lamulo mwampavu, pamenso pa Mulungu na Klistu Yesu na bangeli bake bosankiwa, kuti usunge aya malamulo mopanda kapatulula, osati kuchita kali konse mosanka. ²² Osaika manja pali ali onse mwamusanga. Osa tengako mbali ku machimo ya ali onse muntu. Zisunge oyela weka. ²³ Leka kumwa manzi yeka chabe. Koma, ukazimwako tu vinyu tung'ono chifukwa cha mumala mwako na kudwala-dwala kwako. ²⁴ Ma chimo ya bantu bena ya zibiko poonekela, yabasogolela pamene baenda kuweluziwa. Koma machimo yenangu yama konka kumbuyo. ²⁵ Chimozi-mozi, zinchito zabwino zizibika poyela, koma yenangu siyanga bizike.

Chapter 6

¹ Lekani bonse bali mu ukapolo bapeleke ulemu kuli ba bwana babo. Bayenela kuchita ichi kuti zina ya Ambuye na chipunziso visanyonewe. ² Baja bakapolo bali na ba bwana babo bokulupilila basabataile ulemu chifukwa niba bale. Koma, bayenela kubasebenzela. Chifukwa bakazembe bamene batandiziwila mu ntchito yabo nibokulupilila nafuti bayenekela kubakonda. Punzisa na ku lalikila ivi vintu. ³ Ngati muntu aliyense apunzisa chipunziso chaboza chamene sichivomelezana na chipunziso cha nzelu cha Ambuye watu Yesu Klistu na chipunziso cha umulungu, ⁴ eve nio-zitukumula nafuti kulibe chamene aziba. Alina vofuna vamene sivabwino vofuna vovutana mu kushushana-shushana mau yamene yalengesa vokumbwila, ndeo, kutukwana, voganizilana voipa, ⁵ na kuvutana kwamene sikusila pakati pa bantu bamene bali na nzelu zoipa. Bataya cha zoona nafuti baganiza kuti umulungu ni njila yotengelamo ndalama. ⁶ Umulungu naku nkala okutula ni cha pindu kwambili, ⁷ chifukwa kulibe chamene tinaleta mu ziko ya pansi, nafuti kulibe chamene tizachosamo mu ziko. ⁸ Koma, lekani tinkale bokutula na chakudya na vovala. ⁹ Manje baja bamene bamafuna kunkala bolemela bamagwela muma yeso, mu m'sampa. Bamagwela mu vambili voipa vilako-lako, na mu vonse vamene vimalengesa bantu ku mbila mu kuonongeka. ¹⁰ Kukonda kwa ndalama ndiye koyambila kwa vontu vonse voipa. Bantu benangu bamene bafunisisa ndalama banatengewa kuchosewa ku chikulupililo na kuzilasa beka na zomvesa chisoni. ¹¹ Koma iwe, muntu wa Mulungu, taba ku vintu ivi. tamangila chilungamo, umulungu, kukulupililika, chikondi, kulimbikila, na kunkala odeka mutima. ¹² Chaya nkondo yabwino ya chikulupililo chako chamene chikupulumusa. Gwililila umoyo wamene siusila kwamene unaitaniliwa, wamene unapeleka umboni wabwino pamenso pa baka mboni bambili. ¹³ Nikupasa aya ma lamulo pamenso pa Mulungu, wamene amapasa moyo ku vintu vonse, na pamenso pa Klistu esu, wamene ana peleka umboni wabwino pa menso pa Pontiyasi Pilato, ¹⁴ kusunga lamulo kulibe cholakwa kufikila mpaka kuonekela kwa Ambuye Yesu Klistu. ¹⁵ Mulungu azaonesela kuonekela kwa Klistu pa ntawi yoyenela-Mulungu, odalisika komanso Olamulila Eka, Mfumu wamene atumikila na Mbuye wamene alamulila. ¹⁶ Eve Eka ndiye ali na moyo wamene ulibe malile nafuti ankala mu kuunika kwamene sikufikiwa. Kulibe muntu wamene amuona kapena kukwanisa kumu ona. Kwa eve kunkale ulemu na mpavu yamene si isila. Amen. ¹⁷ Bauze bolemela mu ziko ino kuti basankale bozitukumula nafuti kuti basaike chiyembekezero chabo mu chuma, chuma chamene sichizibika ntawi yake. Koma, baike chiyembekezo chabo muli Mulungu. Eve apeleka kuli bonse chuma cha zoona kuti bamvele bwino. ¹⁸ Bauze kuti bachite vabwino, bankale bolemela mu zintchito zabwino, na kunkala bozipoleka mukupasa nafuti kunkala bofunisisa kugabana. ¹⁹ Munjila iyi bazazi sungila pa beka maziko yabwino ya vamene vibwela, mwakuti bagwililile umoyo wamene siusila. ²⁰ Timoti, chingilila chamene chinapasiwa kuli iwe. Kana vokamba vilibe ntchito na voshushana-shushana vamene vi itaniwa kuti nzelu. ²¹ Bantu benangu balalikila ivi vintu ndipo mukuchita ivi bataya chikulupililo. Leka chisomo chinkale naiwe.

2 Timothy

Chapter 1

¹ paulo, mtumwi wa yesu khristu kupyolera mu chifunilo cha mulungu, kulingana na malonjezo ya umoyo wamene uli mwa yesu khristu, ² kwa timoteyo, mwana okondedwa: chisomo, chifundo na mtendere kucokera kwa mulungu atate ni yesu khristu ambuye athu. ³ niyamika mulungu, wamene nitumikila kuchokera ku makolo yanga, na chikumbu-mtima chabwino, mwamene nikumbukila inu mu ma pempero yanga usiku na muzuba. ⁴ Pamene nikumbuka misozi yanu, nifunisisa kukuonani, kuti ninkhale okondwa. ⁵ nakumbusidwa za chikulupiliro chanu cha zoona, chamene chinali mwa ambuye banu bakazi ba lois na ba mai banu ba eunice, ndipo nisimikiza kuti chinkhala mwa inu futi. ⁶ Ichi ndiye chifukwa chamene nikukumbusani kuti muyashe futi mpaso ya mulungu mwa inu kupyolera mukusanjika manja yanga. ⁷ Pakuti mulungu sanatipase muzimu wa mantha, koma wa mphamvu na chikondi komanso wa kuzileza. ⁸ Manje imwe musankhale na nsoni pa umboni wa mabuye wathu, kapena wa ine, paulo kaidi wake. umalo mwake, gawanani mu mabvuto yake pa uthenga wabwino kulingana na mphamvu ya mulungu. ⁹ Ni mulungu wamene anatipulumusa na kutiyitana na kuitana kwake koyera. anacita izi, sicifukwa cha nchito zathu, koma kulingana na ndondomeko yake na chisomo. anatipasa zinthu izi mwa khristu yesu nthawi ikalibe kufika. ¹⁰ Manje chipulumuso cha mulungu chaonekera pa kuoneka kwa yesu khristu mpulumusi wathu. ni khristu wamene anasiliza imfa na kubweresa umoyo wamene

susila pa kuwala kupitira mu uthenga wabwino. ¹¹ Chifukwa cha ichi, ninasankhidwa kunkhala olalikira mau, mtumwi na mupunzisi. ¹² Pa ichi naine nimabvutika navo. koma nilibe nsoni, chifukwa nimuziba wamene nikulupilira. ninachisimikizo kuti akwanisa kusunga vamene ninamupasa kufika siku ija. ¹³ Sungani chisanzo cha mauthenga ya chikulupiliro yamene munamvera kwa ine, na chikulupiliro na chikondi zamene zipezeka mwa khristu yesu. ¹⁴ Chinthu chabwino chamene mulungu anakupasani, sungani bwino kupyolera mwa muzimu oyera, wamene ankhala mwa ife. ¹⁵ Muziwa izi, kuti bonse bamene bankhala ku asia banachoka kwa ine. mu gulu iyi muli phygelus na hermogenes. ¹⁶ Ambuye acitire chifundo nyumba ya onesiphorus, chifukwa ananisunga bwino ndipo sanachite nsoni na zingwe zanga. ¹⁷ Mumalo mwake pamene anali ku rome, ananisakila kwambiri, ndipo ananipeza. ¹⁸ Mulungu akamucitire chifundo pa siku lija. njira zonse zamene ananithandiziramo ku ephesus, muziwa bwino.

Chapter 2

¹ iwe, mwana wanga, limbikitsidwa mu chisomo chamene chili mwa yesu khristu. ² zinthu zamene munamvera pakati pa mboni zambiri, ziperekeni ku banthu bokulupilika bamene bazakwanisa kupunzisa benangu. ³ Bvutikani na ine, kwati mu silikali wabwino wa yesu khristu. ⁴ Palibe musilikali wamene agwira nchito pamene ali na zinthu zobvuta zambiri za umoyo, kuti akondwerese basogoleri bake. ⁵ Komanso, ngati winangu apikisana pa kutamanga, sapisidwa mphoto pokapo ngati wasata malamulo. ⁶ nikofunikira kuti mulimi olimba pa nchito alandira gawo lake la mbeu poyamba. ⁷ Ganizirani zamene nikamba, pakuti mulungu azakupasani kumvesesa pa zonse ⁸ Kumbukirani yesu khristu, kuchoka ku mbeu ya davide, wamene anaukisidwa kwav akufa. Izi ni kulingana na uthenga wabwino wanga, ⁹ Wamene nibvutikira mpaka kunkhala kwati kawalala mu zingwe. koma mau ya mulungu siyali mu zingwe. ¹⁰ Koteri nipilila zinthu zonse kamba ka iwo bamene ni bosankhidwa, kuti nabeve bapeze chipulumuso chamene chili mwa khristu yesu na ulemelero wosatha. ¹¹ zonena izi ndi zokulupilika: "ngati tafa nayeve, tizankhalaso na moyo nayeve. ¹² Ngati tilimbika, tizalamulira nayeve. ngati timukana, nayeve azatikana, ¹³ ngati ndife osakulupilika, yeve ankhala okulupilika, chifukwa sangazikane yeka. ¹⁴ Pitirizani kuwakumbusa pa zinthu izi. muwachenjeze pamaso pa mulungu kuti sibafunika kuyambana pa mau. chifukwa cha ichi palibe chinthu chapindu. chifukwa cha ichi pali chionongeko kwa iwo bamene amvera. ¹⁵ Muyesese kuzipereka kwa mulungu ngati wamene avomelezedwa, wanchito wamene alibe chifukwa chochitira nsoni, wamene apunzisa mau ya chilungamo. ¹⁶ Pewani zokamba zopanda pindu, zamene zipangisa kuti munkhale kutali na umulungu. ¹⁷ Vokamba vao vizayenda monga gangari. Mwa iwo pali hymenaesus ni philetus, ¹⁸ aba ni banthu bamene baphonya choonadi. Bakamba kuti kuukisidwa kunachitika kudala. Bapindamula chikulupiliro cha benangu. ¹⁹ Koma, maziko yolimba ya mulungu yaimilira. yali na zolembedwa izi: "ambuye aziba wamene ali wake"na "aliyense wamene akamba pa zina la mulungu ayenera kuchoka ku njira zoipa." ²⁰ Mu nyumba yochita bwino, mulibe zikopo chabe za golide na siliva. muli zikopo za mitengo na dothi. zina mwa izi ndi zogwirisa nchito molemekezeka, na zinango nchito zosalemekezeka. ²¹ Ngati winangu azisuka yeka pa nchito zosalemekezeka, ankhala chikopo cholemekezeka. apatulika, chofunikira kwa mwini wake, na chokonzedwa pa nchito zabwino. ²² thabani chilako-lako. funani chiyelo, chikulupiliro, chikondi na mutendere na iwo bamene baitana pa ambuye na mtima oyera. ²³ Koma kanani upuba na mafunso ya ufontini. muziba kuti yamabala mukangano. ²⁴ Kapolo wa mulungu safunika kuchita mukangano. ²⁵ Mumalo mwake ayenera kunkhala odekha mtima kwa aliyense, okwanisa kupunzisa,na ofasa. ayenera kupunzisa mwachilungamo bamene bamushusha. mulungu angabapulumuse kamba ka nzeru za zoona. ²⁶ Bangankhalenso bwino na kuleka musampha wa satana, pamene bagwiriwa kuchita nchito zake.

Chapter 3

¹ Koma zibani ichi: pa masiku yosiliza pazankhala nthawi yobvuta maningi. ² Banthu bazazikonda, bokonda ndalama, bozitukumula, banthota, bonyozela, bosamvera makolo, bosayamika na bopanda chiyelo. ³ Bopanda chikondi chobadwa nacho, wokonda kunyoza, bosazilesa, ba nkhanza, bosakonda zabwino. ⁴ Bamene bazapeleka banza, bamambala, bokonda kusebela kuposa kukonda mulungu. ⁵ Bazankhala na maonekedwe ya umulungu koma mphamvu yake banaikana. chokani pakati pa banthu otero. ⁶ Chifukwa benangu ni banthu bamene bangena mumanyumba na kugwira bakazi bopusa. aba ni bakazi bamene nibozula na machimo elo bamayenda na zilako-lako zambiri. ⁷ Bakazi aba nthawi zonse bamapunzira, koma sibakwanisa kuziba chilungamo ⁸ munjira imozi-mozi mwamene jannes na jambres banaimilira mu njira ya mose. mu njira yamene iyi bapunzisi ba boza bamaimilira kusekeleza choonadi. ni banthu bowonongeka mu maganizo, bosasimikizilika pa chikulupiliro. ⁹ Koma sibazayenda patali maningi. kamba ka kuti upuba wabo uzazibika kuli bonse, monga mwamene chilili kuli bamuna benangu. ¹⁰ koma kwa inu, mwakonkha chipunziso changa, chinkhalidwe, chilingo, chikulupiliro, kupilira, chikondi, kuleza mtima, ¹¹ zobvuta, manzunzo na zamene zinachitika kwa ine ku antioch, pa iconium na ku lystra. ninalimbikira kunzunzidwa. pa zonse, ambuye bananipulumusa. ¹² bonse bamene bafuna kunkhala mwa mulungu mwa yesu khristu bazanzunzidwa. ¹³ banthu boipa na okopela chizankhala chobvuta maningi. bazasokoneza benangu. beve basokonezewa kudala. ¹⁴ Koma kwa inu, nkhalani mu zinthu zamene mwapunzira na kukulupilira mwa mphamvu. muziba kwamene mwazipunzira. ¹⁵ Muziba ati kuchoka pamene munali mwana mwaziba zolembedwa zopatulika. Ivi vikwanisa kukupangani kuti munkhale ba nzeru pa chipulumuso kupyolera mu chikulupiliro cha yesu khristu. ¹⁶ malembo yonse yanauzilidwa na mulungu. ni yaphindu pa chilamulo, pa kutsutsa, pa kukonza ni pa kupunzitsa pa chiyelo. ¹⁷ izi zili tero kuti munthu wa mulungu ankhale okwanira bwino, pa nchito zonse zabwino.

Chapter 4

¹ nipereka chilamulo ichi pamaso pa mulungu ni yesu khrostu, wamene azaweruza amoyo na bakufa, ndipo chifukwa cha kuonekera kwake na umfumu wake: ² Lalikani mau. nkhalani okonzeka pamene zili bwino na pamene sizili bwino. simikizirani, zuzulani, yamikani na kuleza mtima na chipunziso. ³ pakuti nthawi izafika pamene banthu sibazakonda chipunziso chabwino. mumalo mwake bazaitana apunzisi kulingana na zofuna zao. bamene bazamvesa bwino matu yawo. sibazafuna kumvera chilungamo, ⁴ ndipo bazaika matu yawo ku zinthu zaboza. ⁵ koma inu, nkhalani tcheru pa zinthu zonse. bvutikani; gwirani nchito ya uvangeli; chitani nchito yanu. ⁶ chifukwa nithiridwa kudala panja. nthawi yanga ya kuchoka yafika. ⁷ nalimbana nako kulimbana kwa bwino; nasiliza nchito yanga; nasunga chikulupiliro. ⁸ kolona wa chilungamo wasungidwa wanga, wamene ambuye, oweruza oyeru mtima, azanipasa pa siku lija, osati ine chabe koma ku onse bamene bakonda kuonekera kwake. ⁹ chitani zonse zotheka kuti mubwere kwa ine mwa msanga. ¹⁰ Pakuti Demas wanisiya. akonda ziko lino ndipo wayenda ku thessalonika. crescens anayenda ku galatia, tito anayenda ku dalmatia. ¹¹ Luka chabe ndiye ali na ine. Mumutenge Marko mubwere nayeve chifukwa ali na nchito maningi kuli ine pa nchito. ¹² Tichikasi ninamutuma ku Aifeso. ¹³ Chovala chamene ninasiya ku troas na carpus, mubwere nacho pamene mubwera. ¹⁴ alexander waku chipala cha kopa anaonesa zichitidwe zoipa kwambiri pa ine. mulungu azamulipila kulingana na zinchito zake. ¹⁵ Iwe naiwe uyenera kunkhala ochenjera naye, chifukwa anashusha maningi mau yathu. ¹⁶ Pa kuzichinjiliza kwanga koyamba, palibe wamene anaimilira naine. mumalo mwake, bonse banathaba. zisawerengedwe pa iwo. ¹⁷ koma mulungu anaimilira na ine na kunilimbisa kuti mwa ine zokambidwa zikwaniritsidwe mokwanira, nakuti bonse ba mitundu bamvere. ninapulumusidwa mukamwa mwa mukango. ¹⁸ Ambuye bazanipulumusa ku zoipa zonse ndipo bazanipulumusa kamba ka ufumu wa umwamba. kwa iye kunkhale ulemelero nthawi zonse. amen ¹⁹ Mumuposhe priscilla, aquilla, na nyumba ya onesiphorus. ²⁰ Erastus anasala ku corinth, koma trophimus ninamusiya odwala ku miletus. ²¹ Chitani zonse zotheka pamene nthawi yozizila isanafike. eubulus akupasani moni, komanso pudens, linus, claudia, na abale onse. ²² Ambuye ankhole na muzimu wako. Chisomo chinkhole na iwe.

Titus

Chapter 1

¹ Paulo, wantchito wa Mulungu koma futi mutumiki wa Yesu Kristu mu chikulupililo cha bantu ba Mulungu bamene bana sankiwa na mu nzelu za va zoona vamene vivomelezana na umulungu, ² mwa chiyembekezo cha moyo osasila wamene Mulungu, wamene eve samanama, analonjeza pamene kunalibe na mibadwe za ntawi. ³ Pa ntawi yo vomelezewa eve ana onesela mau yake kupitila mu kulalika kwamene ine ninakululupilika kulingana na lamulo ya Mulungu Mupulumusi wati. ⁴ Kwa Tito, mwana wa zoona mu chikululupilo chatu pamozi. Chisomo na mutendere kuchokela kwa ba Tate na Kristu Yesu Mupulumusi watu. ⁵ Chifukwa cha ichi nina kusiya ku Kilete, kuti iwe uike vintu mumalo yake vamene sivali vinasilizika na kunkazikisa ba kulu ba mupingo mu mizinda zonse monga mwamene ine nina kuuzila. ⁶ Mukulu wa mupingo ankale alibe cholakwa, mwamuna wa mukazi umozi, ali na bana bokululupilika bamene sibanga lembewe mulandu wa kusamala kapena bopwanya lamulo. ⁷ Nichofunikila muli olanganila, monga uja oyanganila nyumba ya Mulungu, kuti ankale alibe kolakwa. Safunika kunkala ozitukumula, wakamutima kangono, osatengewa na moba, osati wa ndeo, futi osati ozikonda. ⁸ Koma, afunikila kunkala olandila balendo koma futi muzake wa vintu vabwino. Afunikila kunkala wanzelu, wachilungamo, oyela, futi ozilamulila. ⁹ Ayenela kugwililila mofikapo utenga okululupilika wamene eve ana punzisiwa, mwakuti na eve akwanilise kulimbikisa benangu kupitila mu kupunzisa kwa bwino na ku shusha baja bamene bamu shusha. ¹⁰ Chifukwa kuli bantu bambili bamene sibamvela mau, bamene bakamba vilibe pindu koma futi niba boza, maka-maka pali baja bamudulidwe. ¹¹ Nichofunikila kuba lekesa. Baonongo na banja yonse na mapunziso yabo yo funapo pindu pa kupunzisa vintu vamene vamene beve sibayenela kupunzisa. ¹² Umozi mwa baneneli babo anakamba kuti, "Ba Kilete niba boza ntawi zonse, vinyama voipa, bakamukonda kudya baulesi." ¹³ Kukamba uku nikwa zoona. Mwa ichi, bazuzule kwa ukulu, mwakuti bankale bokonkoloka mu chikululupilo, ¹⁴ osaikilako nzelu ku maganizo ya Ayuda kapena kuma lamulo ya bantu bamene ba chokako ku va zoona. ¹⁵ Kuli baja bamene nibo tuba, vonse vintu nivo tuba. Koma kuli baja bamene bali bo onongeka koma futi bokana ku kululupila, kulibe chotuba, koma nzelu zabo na mitima zabo zina onongeka. ¹⁶ Bama kamba ati

Chapter 1

bamuziba Mulungu, koma bamukana muma chitidwe yabo. Nibo nyansa, bosamvela, koma futi sibo kwanilisa kuchita ntchito ili yonse yabwino.

Chapter 2

¹ Koma imwe, kambani vintu vamene viyendelana na malamulo yokululupilika. ² Punzisa bamuna bakuli kunkala bobwezamo mitima, bozilemekeza, banzelu, ba chikululupilo chabwino, mu chikondi, na futi bopilila. ³ Punzisa bakazi bakulu molinganila kuti bankale baulemu mu mankalidwe, osati bonyozela kapena bakapolo ba moba, koma kuti bankale bopunzisa vintu vabwino, ⁴ naku punzisa bakazi bachichepele kuti bakonde bamuna babo na kukonda bana babo, ⁵ kuti bankale banzelu, boyela, bosunga bwino manyumba, nafuti kunkala bomvela bamuna babo, kuti mau ya Mulungu yasa nyoze. ⁶ chimozi-mozi, limbikisa bamuna bachichepele kuti bakazisebenzesa nzelu zabwino. ⁷ Munjila ili yonse onesesa kuti uzipoleka kunkala chisanzo mu ntchito zabwino. Mu kupunzisa kwako, langiza ubwino, ulemu, ⁸ na utenga wolungama wamene uli pamwamba pa kushushiwa, mwakuti ali onse wamene akushusha achitiwe manyazi chifukwa alibe chilichonse choipa chamene angakambe pali ise. ⁹ Punzisa bakapolo kuti bamvele ba kazembe babo mu vonse, kuti babamvесе bwino osati kushushana nabo, ¹⁰ osati kubabela, koma kulangiza konse kukululupilika, kuti munjila ili yonse banga peleke mayamiko ku mapunziso pali Mulungu wamene ni Mupulumusi watu. ¹¹ Chifukwa chisomo cha Mulungu chaonekela ku bantu kupeleka chipulumuso ku bantu bonse. ¹² Chipunzisa ise kuti tikane umoyo ulibe umulungu na vokonda vamu ziko, na kunkala mozilamulila, molungama, na umoyo wa umulungu mu mubadwe uno, ¹³ pamene tiyembekezela kulandila chiyembekezo chatu chodalisika, kuonekela kwa ulemelelo wa Mulungu wamkulu watu na Mupulumusi watu Yesu Kristu. ¹⁴ Yesu anazipeleka eka chifukwa cha ise kuti ati ombole kutichosa ku omoyo opanda lamulo na kutilenga kunkala otuba bake bantu ba padela bamene bafunisisa kuchita ntchito zabwino. ¹⁵ Kamba pa ivi vintu, limbikisa bantu kuti bachite ivi vintu, nafuti upeleke chizuzulo mwa mpavu. Usa vomeleze muntu ali onse kuti asakutayeko nzelu.

Chapter 3

¹ Bakumbuse kuti bazipeleke ku bolamulila na basogoleli, kubamvelela, kuti bakonzেকেle kuchita ntchito zonse zabwino, ² kuti basanyozele ali onse, basankale bokonzেকেle kuchita ndeo, nafuti kuti bankale botekanya, kulangiza kuzichepesa ku muntu ali onse. ³ Chifukwa naise pa ntawi imozi tinali tinalibe voganiza vabwino na bosamvela. Tinali botaiwa na bakapolo ku vilakolako vosiyasiyana na vozimvesa bwino. Tinankala mu voipa na kuchita kaduka. Tinali bonyansa futi bozondana. ⁴ Koma pamene ubwino wa Mulungu Mupulumusi watu na chikondi chake ku bantu chinaonekela, ⁵ sichinali chifukwa cha zintchito zantu za chilungamo zamene tinali kuchita, koma mwa chsomo mwake anatipulumusa, kupitila mukusukiwa mwa kubadwa kwa sopano na kuwamiyiwa na muzimu, ⁶ wamene Mulungu mosapanda kaso anatila pali ise kupitila muli Mupulumusi watu Yesu Kristu, ⁷ mwakuti mwamene ise tina lembewa opanda mulandu kupitila mwa chisomo chake, tingankale botengako mbali mu chiyembekezo cha umoyo wosasila. ⁸ Uyu utenga niokululupilika. Nifuna iwe ulimbikile pali ivi vintu, mwakuti baja bamene banakululupila muli Mulungu bangankale bosamalila kupeleka kuzi ntchito zabwino. Ivi vintu nivabwino koma futi niva ntchito kuli muntu ali onse. ⁹ Koma kana kushushana kulibe nzelu na va ma mibadwe na ndeo na kushushana pa va malamulo. ¹⁰ Kana ali onse wamene alenga kushushana pakati panu, pamene mwa mu zuzula kamozi kapena kabili, ¹¹ kuziba kuti muntu wamene uyu achoka kunjila yabwino angena muma chimo koma futi azishusha eka. ¹² Pamene ine nizakatuma Alitemas kapena Tikikos kuli iwe, uka endese kubwela kuli ine ku Nikopolis, kwamene naganizila kuti ninkale ntawi iyi yampepo. ¹³ Yesesa njila ili yonse kuti utume Zenasi oimililako bamilandu na Apolosi, kuti basapelebe kali konse. ¹⁴ Bantu batu bayenela kuzipeleka ku ntchito zabwino zamene zipeleka vintu vofunikila maningi, munjila iyi sibazankala balibe pindu. ¹⁵ Bonse bamene bali naine bakusa moni. Bapase moni bonse bamene batikonda muchikulupililo. Chisomo chinkale naimwe bonse.

Philemon

Chapter 1

¹ Ine Paulo, wandende chifukwa cha Khristu Yesu, na m'bale Timoteyo, kwa Filimoni, muzathu wokondewa koma futi wantchito m'zathu, ² na kwa Apiya m'longo wathu, na Akipasi m'silikali m'nzathu, pamozi na mupingo wamene umasonkhana m'nyumba mwako. ³ Leka chisomo chinkale kwa iwe na mutendere wochokela kuli Mulungu Atate bathu na Ambuye Yesu Khristu. ⁴ Nthawi zonse nimathokoza Mulungu wanga nikakuchulani m'mapemphero yanga, ⁵ chifukwa nimamvela za chikulupililo chamene muli nacho mwa Ambuye Yesu na chikondi chamene muli nacho ku banthu bake bonse boyela. ⁶ Nipempela kuti kugabana chikulupililo chanu kunkale kwampavu, kuti munkale bozibisisa mofikapo muvabwino vonse vamene tili navo mwa Khristu. ⁷ Pakuti nankala osangalala nafuti na chitontozo chikulu chifukwa cha chikondi chanu, chifukwa mitima ya banthu boyera ba Mulungu yaukisiwa na iwe, m'bale. ⁸ Chifukwa chake, ngankale kuti ndine olimba m'tima mwa Khristu kukulamulani kuti muchite vamene muyenela kuchita, ⁹ koma chifukwa cha chikondi, nikupemphani m'malo mwake—Ine, Paulo, nkhalamba, ndipo manje m'kaidi wa Khristu Yesu. ¹⁰ Nikudandaulira pa mwana wanga Onesimo, wamene ninabala m'ndende. ¹¹ Pakuti poyamba anali muntu wachabe kuli iwe, koma manje ali wothandizila iwe na ine. ¹² Namubweza kuli iwe, wamene ali m'tima wanga. ¹³ Ningankale wokondwela kuti nimusunge ine kuno kuti akazinisebenzela ine m'malo mwako pamene ine nili mu m'ndende chifukwa cha Uthenga Wabwino. ¹⁴ Koma sininafune kucita chilichonse iwe ngati sunanivomeleze. Sininafune Kuti nchito yako yabwino ichoke mukukakamiziwa koma ichoke mu ubwino wako. ¹⁵ Kapena ni chifukwa cha ichi chamene anapatuliwa kuli iwe kwaka nthawi, kuti unkale naye nthawi yonse. ¹⁶ Sazankala futi kapolo, koma kupambana kapolo, mubale wokondewa. Niwokondeka maka-maka kuli ine, ndiponso maka-maka kuli iwe, ku thupi na mwa Ambuye. ¹⁷ Mwa ichi ngati ndine wosebenzela na iwe pamozi, mulandile eve monga ine. ¹⁸ Ngati anakulakwila kapena ali na nkongole kuli iwe, pasa ine mulandu wankongole iyo. ¹⁹ Ine, Paulo, nilemba ivi na kwanja yanga. Ine neka nizakubwezela nkongole iyo- osanena kuti na iwe uli na nkongole kuli ine weka ya umoyo wako! ²⁰ Inde, m'bale, nileke nipezeko pindu muli iwe mwa Ambuye; lengesa m'tima wanga unkale wokondwela. ²¹ Ine kunkala okulupilila mukumvelela kwako, nikulembela kalata iyi iwe. Niziba kuti uzacita kuchila na vamene nikupempa. ²² Pa nthawi imozi-mozi, nikonzeleko malo yanga yofikilapo, cifukwa niyembekezela kuti kupitila mwa mapemphelo yako, nizabwezewa kuli iwe ²³ Epafra, wandende m'nzanga mwa Kristu Yesu, apeleka moni. ²⁴

Chimozi mozi na Marko, Aristako, Dema, pamozi na Luka, bantcito banzanga.²⁵ Chisomo cha Ambuye bathu Yesu Khristu chinkale na mzimu wako. Amen.

Hebrews

Chapter 1

¹ Kudala Mulungu anakamba na makolo kupitila muli baneneri ntawi zambili namunjila zosiyana-siyana. ² Koma masiku yosilizila yano anakamba naise kupitila mu Mwana Wake, wamene anamusanka kunkala wopyana vinthu vonse. Nikupitila muli uyu wamene Mulungu analenga chalo chonse chapansi. ³ Eve ni kusanika kwa ulemelelo wa Mulungu, ndendende mwamene alili. Eve agwila vintu vonse pamozi kupitila mu mau ya mpavu Yake. Pamene anasuka machimo, anankala pansi ku zanja yake yamanja ya Olemekezeka kumwamba. ⁴ Eve anankala mukulu kuli bangelo monga zina yamene anapasiwa kunkala yopambana kuchila yao, nibandani bangelo bamene Mulungu anauza kuti ndiwe mwana wanga, "lelo nankala Tate wako?" ⁵ Kapena nindani m'ngelo wamene Mulungu anauza kuti, "Nizankala Tate kwa eve nakuti azankala mwana kuli ine?" ⁶ Kumo futi pamene Mulungu abwelesa mwana oyamba mu ziko, akamba kuti, "Bonse bangelo ba Mulungu bafunika kumupembeza." ⁷ Pali bangelo akamba kuti, "Ndiye Wamene alenga bangelo bake kunkala chimbili-mbili." ⁸ Koma kuli Mwana wake akamba kuti, "Mupando Wako wachifumu, Mulungu, ni wamuyayaya. Ndodo ya ufumu wako ni ndodo ya yachilungamo." ⁹ Wakonda chilungamo ndipo wazonda kusakonka lamulo. Mwa ici, Mulungu Wako, akuzoza na mafuta ya chimwemwe kuchilapo banzako. ¹⁰ Poyamba, Ambuye, munaika maziko ya chalo cha pansi. Kumwamba ni chilengedwe cha manja Yanu. ¹¹ Bazaonongeka, koma imwe muzapitiliza. Bonse bazasila monga chovala. ¹² Muzakavipeteka monga chi koti, ndipo vizachinjiwa monga chovala. Koma imwe mukali chimozi-mozi, ndiponso ma siku yanu siyasila. ¹³ Nindani m'ngelo wamene Mulungu anauza pantawi iliyonse kuti, "Nkala ku kwanja yanga yamanja mpaka nilenge badani bako kunkala mupando boikapo mendo yako?" ¹⁴ Kansi bangelo simizimu zotumikila, ndipo botumiwa kukasamalila bonse baja bazalandila chipulumuso?

Chapter 2

¹ Chifukwa ca ici tifunikila kuikao nzelu pa vimene tinamvela, kuti tisa choke kuli veve. ² Ngati utenga uja wamene unakambiwa kupitila muli ba ngelo niwovomelezewa, ndipo macimo yonse na kusamvelela kulandila cabe cilango. ³ Nanga tizataba bwanji ngati tasula cipulumuso cacikulu ici? Nichamene chipulumuso camene cina ulusiwa na Ambuye na kunkazikisiwa na kuli se na bamene banamvela ivi. ⁴ Pa ntawi imozi-mozi Mulungu anacitila umboni, pa ivi ma zisonyezi, vodabwisa ndi va mpavu vosiyana-siyana, ndi popaasa mpaso za Muzimu Woyela kulingana na cifunilo cake. ⁵ Mwa ici, si ku bangelo kwamene Mulungu Anaika pansi pa ulamulo wa ziko yamene ibwela, yamene tili kuikambapo. ⁶ M'malo mwake, wina alinaco cocitila umboni ponena, "Kansi muntu nindani, wamene munamu ikako nzelu? Kapena mwana a muntu kuti mumusamalire eve?" ⁷ Munamupanga muntu wosiyanako pansi pang'ono kupambana angelo; munamuvalika eve na ulemelelo na ulemu. ⁸ Munaika vintu vonse pansi pa mendo yake." Cifukwa ni mwa eve mwamene Mulungu Anaika vintu vonse pansi pau lamuliro wake. Koma manje ise sitiona vintu vone pansi pa ulamuliro wake" ⁹ Komai se tiona eve wamene anaikiwa pansi pa bangelo pa kantawi kang'ono, Yesu, anamwalika ulemu cifukwa ca masauso na imfa yake, kui mwa cisomo ca Mulungu angalabe imfa cifukwa ca ise tonse. ¹⁰ Cifukwa cakuti cinali coyenela kuli Mulungu, cifuka vintu vonse viliko cifukwa cha eve na kupitila muli eve, kubweza bana bamuna bambiri ku ulemelero. Cinali coyenela kuli eve kuapnga eve kunkala ciyambi ca cipulumuso cokwanila kupitila muli kuvutika kwake. ¹¹ Cifukwa bonse babili, uja wamene ayelesa na uja wamene ayelesewa avicosa kumozi cifukwa chakuti eve samvela nsoni kubaita beve kuti abale. ¹² Eve anati "Nizaimba va iwe pakati pa abale banga, ni zaimba va iwe mukati mwa gulu ya bantu." ¹³ Ndiponso, "Ndiza kululupira mwa eve ndiponso, "onani, nilipano na bana bamene Mulungu ananipasa ine." ¹⁴ Cifukwa ca ici, pakuti bana bagabana thupi na magari, bagabana ivi vonse munjira imozi-mozi, kuti kupitila mu imfa eve anaononga eve wamene ali mdyelekezi. ¹⁵ Ici cinali munjila iyi kuti, amasule bonse bamene kupitila mu manta ya imfa, banankala umoyo wao bonse mu ukapolo. ¹⁶ Mu cha zo-ona si bangelo bamene eve atandiza koma mubadwe wa Abrahamu. ¹⁷ Cifukwa chake chinali cofunikila kuli eve kunkala ngati babale bake mnjira zones, kuti ankale mkulu wansembe wachifundo na vintu, va Mulungu kuti ankale wopesesa pa macimo ya bantu. ¹⁸ Cifukwa Yesu mwine anavutika na kuyesewa, akwanisa kuandiza bonse bamene bayesewa.

Chapter 3

¹ Cifukwa ca ici, abale banga boyela, imwe mugabana mumaitanidwe yakumwamba. Ganizani pali Yesu, mutumiki komanso mukulu wansembe wa cipangano catu. ² Enze wokululupilika kuli Mulungu, wamene anamusanka eve, mwamene Mose anali wokululupilika mu munyumba yonse ya Mulungu. ³ Pakuti Yesu ayesewa oyenela ulemelelo ukulu wocila Mose, cifukwa iwo bamene bamanga nyumba alina ulemelelo wocila nyumba yamene. ⁴ Nyumba ili yonse imangiwa na muntu, koma wamene amanga vonse ni Mulungu. ⁵ Cifukwa Mose anali okululupilika monga kapolo mu munyumba ya Mulungu yonse. Kucitila umboni pa vintu vamene vili kukambiwa kusogolo. ⁶ Koma Kristu niwokululupilika ngati mwana wamene ali woyanganila mu Nyumba ya Mulungu. Ise ndise nyumba yake yamene ngati tigwililila ku cilimbikiso na ciyembekezo catu. ⁷ Cifukwa ca ici monga mwamene Muzimu Woyela akambila, “lelo, ngati imwe mwamvela mau yake ⁸ osa yumisa mtima yanu monga muntawi yoyesewa mu cipululu. ⁹ Apa ndiye pamene makolo yanu yana wukila pakuniyesa ine. Pa ntawi ya zaka makumi anai, anaona nthito zanga. ¹⁰ Pa ici, nina kalipa nao mubadwe. Ndipo ninanena kuti, “ntawi yonse bankala boyaiika mu mitima zao. Sibanazibe njila zanga. ¹¹ Monga mwamene ninalapila mu-ukali wanga: ‘beve sibazangena mu chipumulo canga.’” ¹² Cenjelani, abale, kuti pakati panu pasankale wa mutima woipa wosa kululupila, mtima wamene wulikutali na Mulungu wamoyo. ¹³ Koma, limbikisanani wina na muzake siku ndi siku, yamene yo itaniwa kuti lelo. “Lelo,” Kutu palibe pali imwe wamene aza yumisa mutima na cinyengo ca ucimo. ¹⁴ Tili wosebenzela pamozi na Kristu ngati ise tizankala wogwilizana mwa mpavu mu cikululupilo mwa eve kocuka paciyambi mpaka posilizila. ¹⁵ Pali ici, cinakambiwa kuti, “lelo, imwe mukamvela mau yake, musalimbise mtima wanu, monga muwukila.” ¹⁶ Nindani uyo wamene anamvela Mulungu na kumu wukila? Nanga si bonse baja bamene banacoka ku Egipto kupitila muli Mose? ¹⁷ Nanga nindani ana mukalipisa pa zaka makumi anai? Kansi sibaja bamene bana cimwa, matupi yao yanasala mu cipululu? ¹⁸ Kuli ba ndani analapila kuti beve sibazakangena mu chipumulo chake, ngati sikuli baja bamene bana mu ukila eve? ¹⁹ Ise taona kuti beve sibanakwanise kungena mu chipumulo chake cifukwa chosakululupila.

Chapter 4

¹ Mwa ici, kucokela pacipangano coyamba mucipumulilo cake cikali covemeleseka kuimilila cenjelani kuti palibe mwaimwe wamene angazalile. ² Popeza kuti tinauziwa uthenga wabwino monga mwamene banauziliwa. Koma uthenga unalibe pindi kuli baja bamene sibanankale muchigwilizano mucikulupililo nabaja bamene banamvelela. ³ Kuli ise bamene tina kululupila kungena mucipumulo, mwamene ana kambila. "Mwana ninalapila mu ukali wanga, sibazangena mu chipumulo." Chingakale njila iyi, kusebenza kwake kunasilizika kucokela kuciyambi ca ziko. ⁴ Kuliko pa mene anakambapo pasiku Sabata: "Koma, Mulungu ana pumula pa siku ya Sabata kuncito zake zonse." ⁵ Mu malemba aya anakamba nafuti kuti, sibazangena mu chipumulo changa." ⁶ Mwa ici, chisalako kuti benangu bazangena mu kupumula kuja, komanso na baja kudala bamene kunalalikiliwako uthenga wabwino sibana kwanise kungena chifukwa cha kusamvela kwabo. ⁷ Mwa ici Mulungu anankazikisa siku imozi, kui itana kuti "Lelo," pamene anakamba kupitila muli Davide mau yamene yabwezewamo kudala: "Lelo pamene umvela liu yake, usakosese mitima zanu." ⁸ Ngati Yoswa ana bapasa mupulo, Mulungu asembe sanakambepo va siku ina. ⁹ Mwai ici kusala Sabata ya kupumula yamene inasungiliwa bantu ba Mulungu. ¹⁰ Chifukwa wamene angena mu mupulo wa Mulungu eve apumula ku zintchito zake, monga mwamene Mulungu anachitila kuzintchito zake. ¹¹ Mwa ici tiyeni tinkale bofunisisa kungena mu kupumula kuja, mwa kuti kusankale aliyense wamene azagwelamo mu kusamvela monga mwamene bana chitila baja. ¹² Chifukwa mau ya Mulungu yali na moyo komanso niya mpavu na kutwa kuchila lupenga uli onse wokutwa konse-konse. Ima ngena kukwanilisa kupatula moyo na muzimu, pokumanila mafupa na za pakati pa mafupa, komanso ikwanisa kuziba maganizo na malingililo ya kumutima. ¹³ Kulibe cholengewa chamene chingabisiwe pamaso pa Mulungu. Koma, vonse vili po onekela vilibe vovibisa pamaso pa uja wamene tiyenela kuzipendela. ¹⁴ Mwa ici, kuona kuti tili naye wampavu mukulu wansembe wamene anapita mu mwamba, Yesu Mwana wa Mulungu, tiyeni tigwilile chikulupililo chatu. ¹⁵ Chifukwa tilibe wansembe mukulu wamene sakwanisa kutichitila chifundo pa zofoka zatu. Koma, tili naye wamene anayesewapo munjila zonse monga mwamene ise timayeselewa, koma eve alibe chimo. ¹⁶ Tiyeni tiyende mwa chikulupililo ku mupando wachisomo, mwakuti tilandile chifundo nakupezako chisomo chotandizila muntawi yopelelela.

Chapter 5

¹ Pakuti mukulu wansembe, osankiwa kucokela pakati pa bantu, banaikika kucita ncito mumalo mwa bantu pa vintu vamene vikuza Mulungu, kotero kuti apelike mpaso na nzembe cifukwa ca machismo. ² Eve, angacite moleza mtima kuli baja bamene saziba ndipo onamiwa cifukwa eve eka niwopelekewa ku zofoka. ³ Cifukwa ca ici, na eve niwofunika kupeleka nsembe za ucimo wake, monga mwamene amacitila pocitila ucimo wa bantu bena. ⁴ Sikwa eve eka kuti ali wonse atenge uyu ulemu. Koma m'malo mwake, ali woitaniwa na Mulungu, monga mwamene Aaron analiri. ⁵ Mnjira imozi-mozi, angakale Kristu sanazipase eka ulemero pozipanga eka mkulu wansembe, m'malo mwake, eve wamene akamba na eve kuti; "Iwe ndiwe mwana wanga; lelo nankala tate wako." ⁶ Cili monga mwamene anakambila pamalo pena, "Iwe ndiwe wansembe ntawi kosasila." Pata coka mumakalidwe ya Melkezedeki. ⁷ Mu masiku aya ya mtupi yake, Kristu anapeleka vonse m'pempero zopempa mwa kupunda na misozi, kuli Mulungu, kuli uyo wamene akwanisa kupulumusa eve kucokela ku imfa, ndipo anamvela cifukwa ca umoyo wa umulungu. ⁸ Ngakale kuti anali mwana, anapunzira kumvelela kucokela kumavuto yamene anapitamo. ⁹ Anapangiwa wokwanila ndipo anankala, m'malo mwa antu wonse amene amvelela eve, cifukwa ca chipulumuso cosata. ¹⁰ Anaikika eve ndi Mulungu kunkala mkulu wansembe mwa makalidwe ya Melikezedeki. ¹¹ Tili na vambili vokamba va Yesu, koma nivo vuta ku vofotokoza cifukwa mwa makutu yanu yaleka kumvela. ¹² Pakuti pa ntawi ino Munali kufunika kuti nimwe akupunzisani zoyamba za ciyambidwe ca utenga wa Mulungu. Mufunika mukaka, osati cakudya cosheta. ¹³ Cifukwa aliyense wamene akudya cabe mukaka alibe kuziwisisa kufikapo kwa utenga wa cilungamo, cifukwa akali mwana. ¹⁴ Koma cakudya coheta cili ca okula. Aba ndibo bamene cifukwa ca kukula alina kumvesesa wopunzisiwa bwino posiyasiyana zabwino ku zoi

Chapter 6

¹ Mwa ici, tiyeni tisiye kuyamba kwa utenga wa Kristu na kuyenda pa sogolo ku kula. Tisa fake futi maziko a kutembenuka kucoka ku zokufa ntchito ndi chikululupiro muli Mulungu. ² Kapena maziko yo ponzila za ubatizo, kuika manja, kuwukisiwa kuba kufa, na ciweluzo chamuyayaya.

³ Tiza cira naivi vintu ngati Mulungu avomeleza. ⁴ Koma sichokwanilisika kuti beve bamene banali pantawi kuziba, banalabako mpaso ya kumwamba, banali banatengako mbali ya Muzimu Oyela ⁵ Nakulaba mau abwino ya Mulungu ndi mpavu za mubadwe wamene ubwela, ⁶ Bamene banataika-sichokwanilisika kuba bweza kutembenuka. Ni chifukwa beve bali kupacika Mwana wa Mulungu mwa iwo futi, na kumucitisa manyazi mo onekela eve. ⁷ Cifukwa ntaka yamene ima mwa mvula yamene imabwela kabili-kabili pali yeve, na chija camene cima bala mitengo cosebenzela kuli abobamene ntaka ina sebenzewa po-iyi ntaka ilandila daliso yocokela kuli Mulungu. ⁸ Koma ikamela minga na volasa, cilibe ntchito ndipo cili pafupi na tembelelo. Kusilizila kwake niku shokewa. ⁹ Komai se ndise bosimikiza kuti kuli vintu vopambana va kumbali kwanu, imwe bokondewa, vintu vamene vikuza kupulumusiwa, ngakale kuti tikamba munjila iyi. ¹⁰ Chifukwa Mulungu alibe kolakwa. Sanga ibale ntchito zanu na chikondi chamene muna langiza chifukwa cha zina yake, chifukwa muna tumikila bantu bake boyela, komanso muna pitiliza kubatumikila. ¹¹ Tifunisisa kuti aliyense pa imwe alangize ku samalila mpaka kumalizilo, mwa kuti mulenge chikulupililo chanu chinkale chosimikiza. ¹² Ichi chili njila iyi kuti musa chite ulesi, koma bokopela baja bamene kupitilila muchi kulupililo na kupilila bama tengako mbali ku ma lonjezo. ¹³ Chifukwa pamene Mulungu ana peleka lonjezo yake kuli Abrahamu, ana lapa pa eve eka, chifukwa sangalape pali wina mukulu. ¹⁴ Anakamba, "Niza ku dalisa iwe nakukupasa banja ikulu." ¹⁵ Mu njila iyi, Abrahamu anatenga chamene chinalonjezewa pamene anapilila mu kulindila. ¹⁶ Chifukwa bantu bamalapa pa muntu mukulu pali beve. Pa ku siliza kwa mukangano wabo, kulapa kumankala chisimikizo. ¹⁷ Pamene Mulungu anaganizila kuti alangize po onekela kuli baja bolandila lonjezo kusachinja kwa ubwino wa lingo yake, ana simikiza ichi naku lapa. ¹⁸ Anachita ichi chamene kuti mukupitila mwa vintu vivbili vamene sivingachinjiwe-kuti sicho kwanilisika kuti Mulungu aname boza-ise, bamene tinatabila kuchingiliziwa, tizankala nacho chilimbikiso chachikulu kugwililila ku chiyembekezo chamene chaikiwa pa menso patu. ¹⁹ Tilinacho ichi kunkala chintu chogwililila komanso chogwilako cha moyo, chiyembekezo chamene chingena mumalo ya mukati mumbuyo mwa chinyula, ²⁰ kwamene Yesu, wamene ana enda kusogolo kwatu kuti imililako ise. Eve ankala wamkulu wansembe ntawi yosasila kulingana na Melikezedeki.

Chapter 7

¹ Anali wamene uyu Melikezedeki, mfumj ya ku Salemu, wansembe wa Mulungu wa pa mwamba, wamene anakumana naye Abrahamu pamene anali kubwelako ku kapaya ma mfumu na ku mu dalisa eve. ² Kunali kuli eve kwamene Abrahamu ana peleka cha kumi pali vonse. Poyamba, tantauzo ya zina yake ni, "Mfumu ya chilungamo"; koma futi eve ni "mfumu ya Salemu," kutantauza kuti, "mfumu ya mutendere." ³ Eve alibe tate, alibe mai, alibe banja, alibe kuyamba kwa masiku kamena kusila kwa moyo. Koma, alingana na Mwana wa Mulungu, chifukwa ankalilila wansembe ntawi kosasila. ⁴ Onani ukulu wake uyu muntu wamene kolo Abrahamu inapeleka cha kumi pa vintu vonse vamene anatenga ku nkondo. ⁵ Lamulo ifuna kuti bana ba Levi bamene bama landila ntchito ya ba nsembe bayenela kutenga chakumi kuli bantu bonse, kukamba kuti, kuli ba bale babo, ngakale kuti beve, pamozi, bachoka kuli Abrahamu. ⁶ Koma Melikezedeki, wamene mu badwe wake siunachokele kulie beve, analandila chakumi kuchokela kuli Abrahamu, na ku mudalisa, eve wamene analandila ma lonjezo. ⁷ Apa kulibe kukana kuti eve wochepa adalisiwa na mukulu. ⁸ Monga apa, bantu ba moyo wamene umasila balandila chakumi, koma mu chintu chija upelekewa umboni kuti eve ankala na moyo osasila. ⁹ Ndipo, muku kamba uku, Levi, wamene anali kulandila cha kumi, ana peleka cha kumi kupitila muli Abrahamu, ¹⁰ chifukwa Levi anali mu tupi ya kolo yake pamene Melikezedeki ana kumana naye Abrahamu. ¹¹ Manje ngati kunkala ofikapo kunali kokwanilisika chifukwa ndiwe umoji wa nsembe wa a Levi (chifukwa cha ichi bantu banalandila lamulo), nanga nichani chamene chizafunikila kuti wansembe winangu kuti aikiwe kulingana na Melikezedeki, koma kuti asaganiziliwe mukulingana na Aaroni? ¹² Pakuti pamene ubusa wa nsembe unachinjiwa, lamulo na yeve iyenela kuchinjiwa. ¹³ Chifukwa wamene ivi vintu vikambiwapo niwa mutundu wina, kwamene kulibe aliyense wamene anatumikila pa guwa. ¹⁴ Manje onani po-onekelatu kuti Ambuye batu banachokela ku mbadwe wa Ayudah, mutundu wamene Mose sana ichuleko mukukamba pa ba nsembe. ¹⁵ Chamene tikamba nicho onekelatu ngati wansembe winangu ankazikiwa mukulingana na Melikezedeki. ¹⁶ Sichi nali kulingana na lamulo ya kukonka mubadwe wa ku tupi chamene china lenga kuti ankale wansembe, koma chinali kulingana na mpavu za umoyo wamane siusila. ¹⁷ Chifukwa ma lemba yakamba pali eve kuti: "Ndiwe wa nsembe ntawi kosasila kulingana na ndondomeko ya Melikezedeki." ¹⁸ Chifukwa lamulo yaku dala iikiwa pa mbali chifukwa ilibe mpavu komanso ilibe ntchito, ¹⁹ (chifukwa lamulo si inapange kantu kali konse kunkala kofikapo), ndiponso chiyembekezo chopambana chi langiziwa, kupitila muli cheve ti bwela pafupi na Mulungu. ²⁰ Koma sichinali chinalibe kulapa! Benangu bamankala ba nsembe kopanda kulapa, ²¹ koma eve ana nkala wa nsembe pamene Mulungu ana mu uza kuti, "Ambuye balapa ndipo sibaza chinja nzelu zabo: 'Ndiwe wansembe ntawi kosasila.'" ²² Kupitila muli ichi Yesu atipasa chisimikizo cha chipangano chopambana. ²³ Ba nsembe bakudala banali bambili kubapenda, chifukwa imfa inali kubalesa kupitilila mu utumiki. ²⁴ Koma chifukwa Yesu ali na moyo wamene siusila, ali na utumiki wansembe wamene unkazikika. ²⁵ Mwa ichi eve akwanilisa kupulumusa mofikapo bonse bamene bafikila Mulungu kupitila muli eve, chifukwa eve ankalila kuba imililako. ²⁶ Chifukwa chinali choyenela kuti tinkale naye wansembe wa mkulu wa mtundu uyu, wamene ni oyela, alibe cholakwa, otuba, opatulika ku bochimwa, komanso oimisiwa kuchila kumwamba konse. ²⁷ Eve safunikila, kusiyana na bakulu bansembe, kupeleka nsembe siku na siku, kuyambila machimo yake, kukonkapo machimo ya bantu bonse. Anachita ichi kamozi kuimililako bantu bonse pamene anazipeleka. ²⁸ Chifukwa lamulo imaika kunkala wansembe mukulu bantu bamene bali bofoka. Koma mau ya kulapa, yamene yana bwela kukonka lamulo, yana ika Mwana, wamene ana lengewa kunkala ofikapo ntawi kosasila.

Chapter 8

¹ Manje cintu camene tikambapo ni ici: tili na nsembe wa mukulu wamene ankala ku kwanja ya yamanja ya mupando wachifumu wa ukulu mu mwamba. ² Eve ni wa ntchito mu malo yoyela, nyumba yo pempelelamo ya zo-ona yameene Ambuye, osati muntu, anamanga. ³ Pakuti onse mukulu wansembe ayikiwa kupeleka mpaso na nsembe. Cifukwa ca ici ni cofunikila kunkala na cintu cina copeleka. ⁴ Manje ngati Kristu anali pa ziko, asembe siwa nsembe, kupea pali abo bamene bapeleka mpaso monga mwa lamulo. ⁵ Eve atumikila kutengela na citunzi tuzni ca vintu va kumwamba. Cili chabe monga Mose ana cenjezewa kuli Mulungu pamene eve anali kuyamba kupanga nyumba yama pempelo: Mulungu anakamba kuti, “Onesesa kuti iwe upange vonse molingana njila yamene ina langiziwa kuli iwe pa lupili.” ⁶ Koma maanje Kristu apokelela utumiki wabwino, monga mwamene alili eve wapakati wa cilonjezo ca cipangano cabwino, camene cina imilila pama lonjezo yabwino. ⁷ Cifukwa ngati cipangano coyama sizenze copanda colakwa, sikungankalecocitika caciki bili. ⁸ Pakuti pamene Mulungu anapeza colakwa na bantu, anakamba, “Onani, ma siku azabwela – akamba Ambuye – pamene ine niza panga cipangano camanje na nyumba ya Israyeli na nyumba ya Yuda. ⁹ Sicizaka nkala monga cipangano camene ine ninapanga namakolo yabo siku yamene ine ninabatenga pa kwanja kwa wokuba sogolela kucoka mu ntaka ya Igupto. Cifukwa beve sibana mvelele cipangano canga, naine sinina bataileko nzelu- akamba Ambuye. ¹⁰ Pakuti ici ndiye cipangano camene ine niza panga na nyumba ya Israyeli yakapita masiku – akamba Ambuye. nizaka ika ma lamulo yanga mu nzelu zawo, ndiponso niza nkala Mulungu wabo, nabo bazankala bantu banga. ¹¹ Sibazaka punzisana wina na muzake wamucalo cimozi na wina wa abale bake, kukamba, ‘zibani Mulungu.’ Pakuti bonse bazakaniziba ine, kucokela paba ng’ono naku bambili. ¹² Pakuti ine niza kacitila cifundo ku zoipa zawo, nama cimo yabo sinizakaba kululukila.” ¹³ Pakuitana ici cipanganoo “sopano”, ana cilankula cipangano coyamba kunkala cakudala, na pamee ici cankala caku dala na cosila ciza coka.

Chapter 9

¹ Chipanga choyamba nacheve chinali nayo ma lamulo yo pembezela komanso nyumba yopempelelamo ya pa ziko ino. ² Chifukwa nyumba inakonzewa. Chipinda choyamba, mwamene munali poikapo nyali, tebulo, na mukate wa kupezekapo kwake, inaitaniwa kuti malo yoyela. ³ Kumbuyo kwa nyula kunali chipinda china, chamene chinali ku itaniwa malo yoyela. ⁴ Munali guwa ya golide yoikamo vonunkila. Munali ka bokosi ka chipangano, kamene kanali kovalikiwa na golide. Mukati mwake munali kapu yamene inali kusunga manna, ndodo ya Aaroni yamene inashuma, komanso ma buku ya chipangano. ⁵ Pamwamba pa kabokosi ka chipangano, a cherabu ba ulemelelo bamene bana chingiliza chovalila cholipilila zolakwa, chamene sitinga kambepo mofikapo. ⁶ Pamene ivi vintu vinakonzewa, bansembe banali kungena mu chipinda cha kunja kwa pokumanilamo ku sebenza ntchito zabo. ⁷ Koma wansembe mukulu eka ndiye anali kungena mu chipinda chokonkapo, chaka na chaka, koma si anali kungena alibe magari yamene anali kuzipelekela eve eka komanso na machimo ya bantu yosaganizila. ⁸ Muzimu Oyela analangiza kuti ngati pokumanilapo poyamba panali pakalipo njila yongenela mu malo yoyelesa si inali inaonesewa. ⁹ Ichi chinali chilangizo cha ntawi yamene tilipo iyi. Vonse vopeleka na va nsembe vamene vipelekewa sivikwanisa ku konza mitima za opembeza. ¹⁰ Vemve vi ikila nzelu ku vakudya na vakumwa na kusiyana-siyana vakusamba kwa volingana na mwambo, ma lamulo ya tupi kufikila ntawi ya kuikiwa kwa vasopano. ¹¹ Yesu anabwela kunkala wansembe wamukulu wa vintu vabwino vamene vabwela. Ana kupita mokumanilamo mwa kukulu komanso mofikapo mwamene simuna pangiwe na manja ya muntu, yamene siyali ya mu ziko yapansi yamene niyo lengewa. ¹² Sichinali kupitila mu magari ya mbuzi na tu ngómbe tungo'no, koma kupitila mu magari yake ndiye mwamene ana ngenela mu malo yoyelesa kamozi kuimililako bonse na kuba tengela chiombolo cha ntawi yosasila. ¹³ Chifukwa ngati magari ya mbuzi na ya tu ngómbe tungóno na ku tila milota ya ngómbe pali baja bamene banankala na doti kuma bapatula kunkala ba Mulungu kuba suka ma tupi yabo, nanga kuzankala. ¹⁴ kuchilapo njila yabwanji mwazi wa Kristu, wamene kupitila mu Muzimu wamu yayaya anazipeleka alibe kolakwa kuli Mulungu, kusuka mitima zanu kuchoka ku zintchito zakufa kuti musebenzele Mulungu? ¹⁵ Chifukwa cha ichi, eve ni oimililako mu pangano ya manje. Ichi chili njila mwa kuti, chifukwa imfa yankalapo kumasula bonse bamene banali pansu pa chipangano choyamba kuma chimo yabo, bamene baitaniwa bazalandila lonjezo ya kutengako mbali ku zaku landila. ¹⁶ Chifukwa pamene pali chifunilo, imfa ya wamwene analonjeza iyenela kusimikiziwa. ¹⁷ Chifukwa chifunilo chimankala na mpavu pamene pankala imfa, chifukwa ilibe mpavu ngati wamene anai panga akali na moyo. ¹⁸ Mwa ici angakale na chipanga cho yamba sichinali kunkazikiwa ngali kulibe magari. ¹⁹ Chifukwa pamene Mose ana peleka ma lamulo yonse ku bantu, ana tenga magari yq ngómbe na mbuzi, na manzi, na wulu yofela, na hysopo, na kutila pa buku yeve na bantu. ²⁰ Anakamba kuti, "Aya ndiye magari yamene Mulungu aku lamulilani." ²¹ Munjila imozi mozi, ana tila magari pa malo yokumanilamo na vonse vigubu vamene vinali kusebenzesewa mu musonkano. ²² Kulingana na lamulo, vintu vonse kusiyapo chabe tungóno visukiwa na magari. Ngati siku natilike magari kulibe chikululukilo. ²³ Mwa ici chinali chofunikila kuti vitunzi-tunzi va vintu vaku mwamba viyenela kusukiwa na nsembe za nyama. Koma, vintu vaku mwamba vemve vinali kuyenela kuvisuka na nsembe zochilapo. ²⁴ Chifukwa Kristu sanangene mu malo yoyelesa yopangiwa na manja, yamene nichu tunzi-tunzi ya cha zo-ona. Koma anangena ku mwamba kwamene, kuonekela manje pamaso pa Mulungu chifukwa chatu. ²⁵ Sana ende muja kuti akazipeleke kambili, monga mwamene amachitila wansembe wamukulu, wamene amangena mu malo yoyela chaka na chaka na mwazi wa wina. ²⁶ Chifukwa ngati chinali njila iyi, chinali kufunikila kuti akazivutika kwambili kuchokela kuyamba kwa ziko. Koma manje anaonekela pa kusa kwa mibadwe kuti achosepo chimo pa kuzipeleka kwa eve eka. ²⁷ Monga mwamene muntu ankazikiliwa kuti amwalile kamozi, kukonkapo nikuweluziwa, ²⁸ chimozi-mozi, Kristu anapelekewa kamozi kuchosapo machimo ya bantu bambili, komanso azaonekela kachibili, osati kukonza chimo, koma kupulumusa bonse bamene bamu lindila.

Chapter 10

¹ Pakuti lamulo ni citunzi-tunzi cabe ca vintu vabwino vamen vizabwela, osati vamene vamene. Beve bamene bamafika kuli Mulungu sangakale wokonzeka bwino nsembe yamene ija ansembe amabwelesa caka na caka mobwezela. ² Mnjira ina, kupeleka nsembe sembe kupeleka? Pakuti baja wopembeza bamene banasukiwa kamozi, cabe sembe balibe cikumbumtima ca uli ucimo. ³ Koma ni nsembe zija ciliko cikumbuso ca macimo caka na caka, ⁴ Pakuti sicoteka magari ya ng'ombe na mbuzi kucosa macimo. ⁵ Pamene Kristu anabwela pano pa ziko, anakamba kuti, “nsembe nazopeleka simuzifuna imwe, koma tupi mwani konzela ine.” ⁶ Na zopeleka zoshoka na zopeleka za ucimo simunazikonde imwe. ⁷ Ndipo anati, “onani, ine nilipano mwamene zinalembelewa za ine mu buku kuti incite, Mulungu, cifunilo canu.” ⁸ Poayamba anakamba eve kuti, “sizinali nsembe, kapena vopeleka, kapena vopeleka voshoka, kapena nsembe zaucimo yamene munafuna. Nafuti, simukondwela navo.” Iyi ndite nsembe yamene ipelekewa kulingana na lamulo. ⁹ Ndipo eve anati, “onani, apa nizacita cifunilo canu.” Anacosa cocita coyamba kuti cocita cacibili cinkazikike. ¹⁰ Mwacifunilo ici, tankala wosambisiwa kupitila mu kupelekewa kwa tupi ya Yesu Kristu kamozi cabe kuli bonse. ¹¹ Siku na siku wansembe ali-onse anali kuimilila nakutumikila, nakupeleka nsembe imozi-mozi mobwezela-bwezela-nsembe yamene si-inali kukwanisa kucosa macimo. ¹² Koma pamene Kristu anapelekewa kwa ntawi yonse nsembe yamacimo, eve ana enda kunkala pansi, ku kwanja ya manja ya Mulungu. ¹³ Anali kuyembekeza kufwikila adani aikiwe codyakapo camendo yake. ¹⁴ Pakuti pa copeleka cimozi anakwanisa kwantawi zones baja bamene banasambisiwa. ¹⁵ Muzimu Oyela na eve ama cita umboni kuli ise. Poyamba anakamba kuti, “¹⁶ “Ici ndiye cipangano camene nizapanga nabo, pambuyo pa masiku yaja, bakamba Ambuye.” Nizaika ma lamulo yanga mumitima zao nafuti nizayalemba pa nzelu zao.” ¹⁷ Ndipo banaikilapo, “macimo na vopeleka vanu sinizavikumbukila nafuti.” ¹⁸ Manje paliponse pamene pali cikulukilo pa ivi, palibe kupeleka nafuti nsembe ya macimo. ¹⁹ Cifukwa ca ici, Abale, tili na cisimikizo kungena mumalo yoyela maningi mu magari ya Yesu. ²⁰ Icindiye coyamba na njira ya moyo yamene anaikazikisa kuli ise kupitila mu cinyola camapinda, camene cili mwa tupi yake. ²¹ Cifukwa tili naye mkulu wansembe woyanganila nyumba ya Mulungu ²² Tiyeni tibwele na mitima ya zo-ona muchikululupiro namu cisikimizo cokanila nqa matupi yosambisiwa na manzi yalibe doti. ²³ Tiyeni tigwilise kosakaikila ku ciyembekezero camene timavomela na pa kamwa patu, cifukwa eve wamene anatonjeza niwokululupilika. ²⁴ Tiyeni tione mwamene tingalimbikisilane umozi na muzake mucikondi na muncito zabwino. ²⁵ Tiyeni tisaleke muku kumana kwatu pamozi, mwamene bena bamacitila. M'malo mwake, limbikisanani kwambiri umozi na muzake na muvonse kwambiri, pamene muona masiku yafika pafupi. ²⁶ Pakuti ngati tipitiliza kucimwila dala pambuyo polandila utenga wa zoona, nsembe ya ucimo si izapasiwa kwa ise. ²⁷ M'malo mwake, kuli cabe ciyembekezo cimozi coyofya ca ciweluzo, ndiye cimoto cikulu camene cizaononga adani bonse ba Mulungu. ²⁸ Ali onse wamene alibe cifundo pa umboni wa bantu babili kapena batatu. ²⁹ Molingalila nikotani kukula kwa cilango mwamene cizankalila kuli uja wapepusa Mwana wa Mulungu, wamene ayesa ci pangano ca mwazi, kunkala cosayela-mwazi wamene unamuyelesa-ndipo anyoza Mzimu wa cisomo? ³⁰ Cifukwa timuziba eve wamene anakamba kuti. “Kubwezela nikwanga; Ine nizabwezela.” Ndipo futi, “Ambuye bazakawelua bantu babo.” ³¹ Nicintu coyofya kugwa nakucoka mumanja ya Mulungu wa moyo!” ³² Komma kumbukani masiku yakumbuyo, pamene munaziba, mwamene munavutikila mumasauso yakulu. ³³ Munapelekewa mukusausiwa ndipo Munali kugabana masauso na baja bamene banapitamo. ³⁴ Pakuti Munacitila cifundo baja bamene banali womangiwa ndipo munacilandila na cimwemwe kupokewa kwa katundu wanu. Munaziba kuti imwe muli na yabwino nay a muyayaya katundu. ³⁵ Mwa ici musataye cikululupiro, camene cili na mpoto ikulu. ³⁶ Pakuti imwe mufunika cipiliro kuti pamene mucita za cifunilo ca Mulungu, muzalandila camene cinalonjezewa. ³⁷ “Pantu mwa kantawi kang'ono, wamene abwela azabwela mosacedwa. ³⁸ Abo bacilungamo banga bazankala na moyo mwa cikulupiliro. Ngati bazabwelela kumbuyo, moyo wanga suzakondwela nabo.” ³⁹ Koma ise sitili monga baja bamene bazabwelela ku cionongeko, koma ise tili pali baja bamene bali na cikululupiro na wosunga moyo zabo.

Chapter 11

¹ Manje chikhulupililo nikunkhala wa simikizila pa vinthu vamene muyembekeza, zosaoneka. ² Chifukwa ca ici makolo batu anakhala ba chikulupililo. ³ Mwa chikulupililo timvesesa kuti chalo china lengewa na wamu Mulungu mo lamulila, kuti manje vo oneka vinapangiwa mopanda zoneka. ⁴ Mwa chikulupililo Abeli anapeleka kwa Mulungu nsembe ya bwino yoposa ya Kain, mwa ici anapezeka wolungama ndipo Mulungu anakamba bwino za eve chifukwa cha vopeleka vake, mwa chikulupililo Abeli akamba, ngakhale kuti anafa. ⁵ Ndi mwa chikulupililo kuti Enoki anatengewa kumwamba kuti asaone infa. " Akalibe kutengewa ku mwamba anachitila umboni kuti anakondwelesa Mulungu. ⁶ Manje mopanda chikulupililo na chovuta, kukondwelesa, ise. Chifukwa ca ici cho chofunikila kuti aliyense amene abwela kwa Mulungu akhale na chikulupililo kuti aliko kuti ni eve apasa mpaso kwa eve amene amusakila. ⁷ Ndi mwa chikulupililo kuti Nowa, ngakhale kuti anali anapasiwa mau a Mulungu pa vinthu vosaoneka, na pocita mantha, ya Mulungu apanga combo kupulumba abanja yake. Pakuti ici azudzula ziko lapansi anakhala mwana wa chikulupililo. ⁸ ndi chikulupililo kuti Abuham, pamene anayitaniwa, anamvelela napita kunja kwa mene anali ku pasiwa vinthu cholowa. Anayenda kunja, osaziba kumene anati apite. ⁹ Ndi mwa chikulupililo kuti anakhala mdziko ionjezewa imene sinali ya kwao. Anakhala mu msasa na Isaki na Yokobo, Abale ana achiyembe chimodzi. ¹⁰ Pakuti analikuyembekezela kuona mdzinda wamaziko opanga naku mangiwa na Mulungu. ¹¹ Mwa chikhulupililo - Sara eve anali cumba- analandila mphamvu nakukhala na mimba ina pitapita nthawi yobala, chifukwa ana khupilila eve amene anamilonjeza. ¹² Manje, cokela munthu amene uyu ali pafupi kufa, anabadwa ambili ngati nyenyezi mu mtambo zosawelengeka monga ni muchanga. Mumbali mwa mangi mana. ¹³ Chinali mwa chikulupililo onse anafa osalandila cilonjezo. Malo mwake ata waona patali nawapasa moni patali, anavomela kuti anali alendo ndi obisama pa ziko lapansi. ¹⁴ Pakuti banthu amene akamba mau yaso afuna malo ponkhala. ¹⁵ Ngati aganiza za ziko yamene banayendako, anakankhala na mpata wobwelelamo. ¹⁶ Koma mene zili, afuna ziko yabwino, kuti ichi, chifukwa ichi, nicha ku mwamba. Mulungu alibe manyazi kuchedwa Mulungu wao, pakuti apanga mzinda waiwo. ¹⁷ Chinali mwa chikulupililo kuti Abuham, anayesewa, anapeleka Isake, anali mwana wake mwana eka amene anapeleka, eve, amene analandila eve amene monga mwa molonjezo. ¹⁸ Kwa Abuham cinali cinakambiwa, " Nikuchokela kwa Isake kuti mbadwe uzayitaniwa." ¹⁹ Abulham anaganiza kuti Mulungu akwanisa kuusa Isake kuchokela ku infa, kukamba moyelekeza, kunali kwa beve analandila. ²⁰ Chinali mwa chikulupililo mwa vinthu vobwela kwa Isake adalisa Yakobo na Esau. ²¹ Ndi mwa chikulupililo kuti Yakobo, pamene ali kufa, adalisa onse ana amuna a Yosephe. Yakobo anapempeza, akupunzila pamwamba pa vinthu vake. ²² Mwa chikulupililo kuti Yosephe, pamene analipafu kufa ana kamba pa kucoka kwake kwa ana Isreal ku Egpito , ndipo anawauza zocita pa mafupa yake. ²³ Mwa chikulupililo kuti Mose, pamene anabadwa, anabisiwa kwa miyezi itatu ndi makolo ake cifukwa anona kuti anali mwana okongola kwambili. Sanaope Mfumu ulandililo wake. ²⁴ Mwa chikulupililo Mose, pamene akula anakana kuitaniwa mwana wa mkazi wa falao. ²⁵ Anasankha kubvutisiwa ndi anthu ake a Mulungu koposa ku kondwela na mkondwelesa za ucimo kwa ka nthawi. ²⁶ Ana ganiza kuti kubvesewa nsoni paza Kristu kuli kopambana cuma koposa cuma za mu Egpito. Anaika maso pa mpaso yake. ²⁷ Ndi mwa chikulupililo Mose anacoka ku Egpito. Sanaone ukali wa Mfumu, analimbikila monga ngati ali atamuona amene osaoneka. ²⁸ Ndi mwa chikulupililo kuti anasunga pasika nakuwaza kwa magari, kuti kuononga kwa ana oyamba kusakhuze ana aesilachi oyamba. ²⁹ Mwa chikulupililo anapita pa manzi pa nyanja yamatete monga ngati pambali po yuma. Pamene a Egpito anayesa kucita izi, anamila mu manzio. ³⁰ Ndi mwa chikulupililo kuti chipupa ca Jeriko chinagwa, Athama kuizunguluka masiku asani ndi awili. ³¹ Ndi mwa chikulupililo kuti Rahabu ule sanafe ndi banja osamvelela chifukwa ana landilila anthu ozonda mzinda mwa mtendele. ³² Nanga nivichani ningakambe apa, pakuti nthawi sindilola ngati ningakambe za Gedioni, Barak, Samson, Jefitali, Davidi, Samuel ndiponso kunena pa aza aneneri. ³³ Zinali mwa chikulupililo anali agonjesa maufumu, anacita ku lungamo, ndipo analandila malonjezo. Analekesa pakamwa pa mkango, ³⁴ a zimya mphamvu ya mulilo, bataba kunolakwa lupanga, anacilisiwa ku matenda yonse, anankhala amphamvu mu nkondo, ana gonjeza adani alendo ankhondo. ³⁵ Azimai analandila ba kufa kupitila mu ciukiso. ³⁶ Ena ana menyewa, osalandila kumasuka, kuti amilile mphamvu ya ociukiso yabwino, kumangikwa naku ponyewa mndende. ³⁷ Ena ponyewa miala. anadulilwa pa wili. Anapayiwa nalupanga. Anayenda mu vikumba va nkhusa na mbuzi. Anali anthu ofuma fuma, ndiku nzunzika, anabvutisiwa. ³⁸ Dziko silinali ya bwino kwa eve. Anali kuyenda-yenda mu chipululu namu mapili, godi namu mgodi. ³⁹ Ngankhale kuti anthu awa anali ovomelekezewa na Mulungu chifukwa cha chikulupililo, sana landile lonjezo. ⁴⁰ Mulungu anakonzelatu za bwino za ise, kuti kulibe ise, ziko ife sizizakhala zo fikapo.

Chapter 12

¹ Chifukwa cha ici, ifenso, popeza tizinguluziwamanthu ambili ochitila umboni, tileke colemagiliyonse cimatiyele kucimo, mwamsanga, tiyeni tamanga na kupilila luwilo yamene ali pa sogolo pa ise. ² Tiyene tiyanganile kwa Yesu, anayamba wokonza bwino chikulupililo. Pakuti cimwemwe cinaikika pa iye, ana pilika pa mtanda, anacitisiwa manyazi anakhala pa zanja la mpando wa cifumu wa Mulungu. ³ Tsopano ganizani pa eve, amene apilila kususana kocokela kwa ocimwa kwaeve yeka, kuti musabvutike naku teya mtima. ⁴ Ukalibe kukanapo kapena kulimbanapo na ucimo kufika pamyeso wocosa mwazi; ⁵ Ndipo waiwala cilimbikitso camene ndi nakupa ngati bana banga: " Mwana wanga usaganizile capafupi ku langiwa na Ambuye kapena akubvutisa pamene ulangiziwa na eve. ⁶ Chifukwa Ambuye ama langa muntu wamene bakonda, komanso bamalanga mwana aliyense wamene bamalandila. ⁷ Pakuti Ambuye alonga aliyense amene amukonda, amlanga aliyense amene amulandila kwa eve. Pilila masauso ngati ana ake. Pakuti ni mwana bwanji amene atate ake sammulonga? ⁸ Koma ngati ulibe cilangizo cimene anthu onse agawana, ponepo ndipo ana amuchigololo osati ana ake amuna. ⁹ Mopitilila, tilinao atate anthu akuthupi amatilonga ndipo timabapasa ulemu. Koposa kotani kugonjela kwa atate anthu aku uzimu ndi wa moyo? ¹⁰ Azi tate anthu ati longa kwa nthawi in'gono cabe pakuti anaganizila ni kwa bwino. Koma Mulungu atilanga ise kwa ubwino wathu, kuti tigabane mu ciyelo cake. ¹¹ Kulibe cilango camene cipasa cimwemwe, koma kupasa kubaba. Koma posilizila cipereka cipatso ca mtendere ca ciyelo kwa eve amene aphunzisiwa naicho. ¹² Mwa ici limbikisani manja yanu oyondolokawa nkhangono zana zofoka. ¹³ Pangani njila zanu za mendo yanu, kuti colemala sicigafalilala koma ku cilisiwa. ¹⁴ Fumisisani mtendele na chiyene na ciyelo pakuti popanda izi kulibe azaona Ambuye. ¹⁵ Onesesani kuti kulibe amene uso weka cisomo ca Mulungu, kuti palibe njila ya ukali izakula mpaka ku mabvuto, kuti ambili saza onongeka nacho ichi. ¹⁶ Nkhale mozi wa cigololo, kapena wa manyozo, ngati Esau, amene mwa chakudya anagulisa ukulu wake wobadwa nao. ¹⁷ Ziwa kuti papita izi pamene ana funa kutenga kupyana madaliso ake, anakaniwa cifukwa kunalibe mwai wolapa, nga khale kuti analila nachosa misozi. ¹⁸ Pakuti simunabwele ku lupili yamene inga gwililiwe, lupili ya yoyaka mulilo, mdima, yabili na cimphepo. ¹⁹ Simunabwele ku lupenga yolila, kapena ku liwu yamene ikamba mau yamene omvela apempa kuti osati mau ena anenewa kwa eve. ²⁰ Pakuti sunakwanise kusunga camene anakulamulila: " Ngakhale nyama ekagwila lupili ifunika ku ponyewa maila." ²¹ Malo yoyofia yamene Mose akamba, anacita mantha naku njejemela." ²² Koma mwabwela ku lupili ya Zion na muzinda wa Mulungu wa moyo, Jerusalemu wa ku mwamba, na zikwi khumi ya angelo mu ku kondwela. ²³ Mwa bwela mu musonkano wa ana obadwa oyamba, amene a lembewa ku mwamba. mwabwela kwa Mulungu, oweluzi wa zonse, ku mzimu wa cilungamo, eve apangiwa bwino. ²⁴ Mwa bwela kwa Yesu, amene ankhala pakati pa cipangano casopano, naku waza kwa mwazi wa bwino wosiyana na wa Abeli. ²⁵ Yanganani kuti simukana amene akamba. Pakuti sanatawe pamene anakana amene ana wa cenjeza pa ziko lapansi, mwa pang'ono muzathawa ngati mwaleka kukamba amene acenjeza za ku mwamba. ²⁶ Pa nthawi ina , liwu yake inagwendeza ziko. Koma tsopano alonjezawa kuti, "Kamozi kanthu imozi ndizagwendeza ziko osati ziko yeka, koma mumwamba." ²⁷ Mau awa, " kwa kamazi kutanthauza kucosa zinthu izo zamene zigwendezeke. Ndiye ici , pa zinthu zamene sizingagwendezeke ziza nkhalu. ²⁸ Tsopano, landilani ufumu wamene sunga gwendezeke, tiyeni tiyamike mu njila iyi yopempeza Mulungu na ulemu na mantha. ²⁹ Pakuti Mulungu wathu ndi mulilo wothantha.

Chapter 13

¹ Lekani cikondi ca ubale cipitilile. ² Musaibale kulandila alendo. Pakuti pakucita ici, ena analandila angelo mosaziwa ici. ³ Kumbukani amudende monga ngati munamangiwa pamozi. kumbukilani amene abvutisiwa nagti kuti muli nao mu thupi. ⁴ Lekani chikwati cilemekeze na onse, lekani pogona pa okwati pankhale poyela, pakuti Mulungu azaweruza anthu aciwelewele naba cigololo. ⁵ Muma nkhalidwe anu musa nkhole okonda ndalama. Khutilani nazo zamene muli nazo, pakuti Mulungu eve yeka akamba, " sizacokapo kapena kukusiyani imwe." ⁶ Tiyeni tinkhale okhutila kuti tinkhale namphamvu kukamba. "Ambuye ndi mthandizi wanga ; Sinidiza yayopa iyayi. Nichani camene munthu anga cite kwa ine? " ⁷ Ganizilani Asogoleli anu, amene akamba mau a Mulungu kwa inu, ganizilani pa zoturuka zake mu ma citidwe awo, akopeleni eve cikhulupililo cao. ⁸ Yesu Kristu ali cimozi lelo na mailo ndipo nthawi zonse. ⁹ Musatengewe nama phunziso ya cilendo. Pakuti cili ca bwino kuti mtima ukhale wolimbisiwa ndi chisomo , osati na cakudya vimene silithandiza amene ayenda na ¹⁰ navo. Tili nayo guwa yamene amene atumika mukati savomelezewa kudya. ¹¹ Pakuti magazi ya nyama yopaiwa cifukwa ca macimo ibwelesa wa na wansembe mkulu ku malo oyera, pamene ma thupi awo kunja kwa msasa. ¹² Cifukwa cace Yesu anasausidwa kunja kwa mzinda pa colowela, kuti asuke banthu kupitila mu magazi yake. ¹³ Tiyeni manje tiyende kuli eve kunja kwa msasa, monyamula nsoni. ¹⁴ Pakuti tilibe malo okhalilila pano. mmalo mwake , tiyembekezela eve amene afunikila ku bwela. ¹⁵ Kupitila muli eve, manje, tikazingopereka nsembe za matamando kuli Mulungu, matamando yaci paso ca milomo yathu yamene ezindikila zina yake. ¹⁶ Tiyeni manje tisaibale kucita bwino naku gawana, ndi mwa nsembe njila iyi yamene Mulungu akondwela yao. ¹⁷ Mvelelani na kuzipeleka kuli asogoleli anu , pakuti akuyanganilani mioyo yanu ngati awo amene azapeleka umboni, mvelanni kuti asogoleli anu acite ici na cimwemwe, koma osati molila, zamene zizankhala zopanda nchito kwa imwe. ¹⁸ Timphempeleni ise, tili na cisimikizo kuti mitima yantu ili yo masuka kuti tifunisisa kunkhala bwino mu zonse. ¹⁹ Nikulimbisani imwe kuti mupitilize kucita izi, kuti nibwele futi uko mwamsanga. ²⁰ Manje Mulungu wa mtendele, amene ana bwelesa akufa ku moyo mbusa wa nkosa, Ambuye Yesu, mwa mwazi wa cipangano camuyayaya, ²¹ akupaseni mphamvu imwe yazonse za bwino kuti mucite cifundo cake, kusebenza muli ise comvesa bwino kuli eve. Tipitila muli Yesu Kristu kuli eve ku nkhole ulemelelo nthawi zosasila. Amen. ²² Manje nikulimbisani imwe abale, musa khumudwe na mau yacilimbikiso yamene yalembewa kwa imwe mwa pang'ono. ²³ Ziواني kuti mbale watu Timoteo masulika pamozi na eve akabwela mwamsanga tizakuonani. ²⁴ Pelekani moni kuli basogoleli banu bonse na bonse banthu aMulungu boyela. Baku Itali bakupasa moni. ²⁵ Cisomo cinkhole na imwe bonse.

James

Chapter 1

¹ Yakobo, kapolo wa Mulungu komanso wa Ambuye Yesu Kristu, kuli mitundu twelofu ili mu kunjani: moni. ² Chioneni kunkala cimwemwe, abale, pamene mupita muma vuto yosiyana-siyana. ³ Muziba kuti kuyesewa kwa chikulupiliro chani chilenga kupilira. ⁴ Lekani kupilira kusilize ntchito yake, mwakuti munkale ofikapo komanso bokwanila, bosapelela kali konse. ⁵ Koma ngati wina mwa imwe afuna nzeru, mulekeni apempe kuli Mulungu, wamene amapeleka mosachita kaso komanso mosakalipira baja bamene bamupempa, ndipo azamupasa. ⁶ Koma lekani apempe muchikululupiro, mosakaikila kalikonse. Chifukwa aliyense wamene akaikila ali monga funde yapa manzi chamene chiyenzewa na chi mpepo komanso chizungulusiwa. ⁷ Chifukwa uja muntu asaganize kuti azalandila kalikonse kuchokela kuli Ambuye. ⁸ Uyu muntu ali na maganizo yabili, ogwedezeke munjila zake zonse. ⁹ Mulekeni osauka mubale azitukule mumalo yake, ¹⁰ koma eve olemela mumalo mwake yapansi, chifukwa azakamwalira monga luba yamusanga muma uzu. ¹¹ Zuba imaima na kupya kwake na kuyumisa ma uzu. Luba imagwa, komanso nakuwama kwake kuonongeka. Munjila imozo-mozi, eve olemela azasila pakati pa ulendo wake. ¹² Odala ni uja muntu wamene apilira mu kuyesewa kwake. Chifukwa pamene akwanisa kusiliza kuyesewa kwake, azalandira kolona ya moyo, yaene inalonzeweka kuli baja bakonda Mulungu. ¹³ Osaleka muntu aliyense pamene ayeseuwa kukamba, "Ine Mulungu aniyesa," chifukwa Mulungu samayeseuwa na chimo, kapena eve kuyesa ucimo muntu aliyense. ¹⁴ Koma muntu aliyense ama yesewa na zofuna zake, chamene chimamu chosapo naku muyesa. ¹⁵ Pochoka apo pamene chofuna chake chichitika, chima bala chimo, ndipo pamene chimo ikula kufikapo, ibala imfa. ¹⁶ Osanamiwa, abale banga. ¹⁷ Mpaso ili yonse yabwino kufikapo ichokela kumwamba. Imachokela kuli Atate baku unika. Kuli eve kulibe kuchinja kapena chimvwilimvwili chochinja. ¹⁸ Mulungu

anasanka kubala is kupitila mu mau yazoona, mwakuti tinkale monga vipaso voyambba muvonse vintu vamene anapanga.¹⁹ Imwe muziba ivi, abale banga bokondewa: lekani untu aliyense ankale wotamanga mukumvela, ochedwa muku kamba, komafuti ochedwa kukalipa.²⁰ Chifukwa ukali wa muntu si-ulenga chilungamo cha Mulungu.²¹ Mwa ici chosani vonse vidoti vau chimo na kuzula kwa uchimo. Mukuzichepesa landilani mau yoshangiwa, yamene yakwanilisa kupulumusa moyo zanu.²² Nkalani bochita mau osati bomvela chabe, kuzinamisa mweka.²³ Chifukwa ngati muntu aliyense ni-omvela mau koma osachita, ali monga muntu wamene alangana pamenso pake mu mila.²⁴ Amaziyangana eka naku enda koma sipapita ntawi aibala mwamene aonekela.²⁵ Koma muntu wamene ayanganisisa mosamalila mu lamulo yofikapo yaufulu, naku pitiliza kuchita ichi, osankala chabe omvela wamene amaibala, uyu muntu azadalisika mu zintchito zake.²⁶ Ngati muntu aliyense aziganizila kuti niwa chipembezo, koma sasamalila mau yake, anama mutima wake, ndipo chipembezo chake chilibe pindu.²⁷ chipembezo chau dongo komanso chopanda kolakwa pamenso pa Mulungu na Atate batu ni ici: kutandizila baja balibe batate babo na bazimai bofedwa muma vuto yabo, na ku zisunga opanda kolakwa muziko.

Chapter 2

¹ Abale, musagwile chikululupiro muli Mbuye watu Yesu Kristu, Mbuye waulemelelo, na kapatulula kuli benangu.

² Ganizilani kuti wina angena mu musonkano wanu avala na mpete ya golide na vovala vabwino, komanso mwangena winangu osauka ovala vovala va doti. ³ Ngati walangana pa uja muntu ovala vovala vabwino naku muuza kuti, "Nipempa kuti munkale apa pabwino," komafuti muuza uja muntu osauka kuti, "iwe imilila paja," kapena, "nkala pansu pa mendo yanga," ⁴ sindiye kuti muweluzana pamweka? Nanga simunankale oweluzana nama ganizo yoipa? ⁵ Mvelani, abale banga bokondewa, kansi Mulungu sanasanke beve bosauka bamu chalo kunkala bolemela muchikululupilo komafuti kunkala bopyana ufumu wamene analonjeza baja bomukonda? ⁶ Koma onani mwanyozela bosauka! Kansi sibamene bolemela bamene bamaku vutisani? Sibamene bamaku peleka ku bwalo yamilandu? ⁷ Sibamakunyozele zina yanu yamene imwe mumatengako mbali? ⁸ Koma, ngati mufikilisa lamulo ya chifumu, kulingana na malemba, "Ukonde mzako monga uzikondela iwe weka." ucita bwino. ⁹ Koma ngati ucita kapatulula ku bantu bena, ucimwa, ndipo iwe uweluziwa na lamulo kunkala opwanya lamulo. ¹⁰ Aliyense wamene akonka lamulo yonse, koma alakwa munjila imozi chabe, aweluziwa kunkala olakwa kuti apwanya lamulo yonse. ¹¹ Chifukwa wamene anakamba kuti, "Osachite chigololo," anakamba futi, "Osapaye." Ngati suchita chigololo, koma upaya, wankala opwanya lamulo. ¹² Mwa ici kambani na kuchita monga baja bantu bamene bazaweluziwa kupitila mu lamulo ya ufulu. ¹³ Chifukwa chiweluzo chimabwela chilibe cifundo kuli baja bamene balibe chifundo. Chifundo chima chila chiweluzo ¹⁴ Pindi ili pati, abale, ngati muntu akamba kuti ali na chikulupiliro, koma alibe zintchito? Nanga chikululupiro ici chinga mupulumuse? ¹⁵ Ganizilani kuti mubale kapena mulongo ovala vovala voipa komafuti alibe vakudya va iyo siku. ¹⁶ Ganizilani kuti wina pakati panu amuuza kuti, "uyende bwino, unkale otuma koma futi udye." Ngati sunamupase vintu vofunikila pa tupi, ivo nivabwino bwanji? ¹⁷ Chimozi-mozi chikulupiliro pacheka, ngati chilibe zintchito zokonkapo, nichakufa. ¹⁸ Koma winangu angakambe kuti, "uli na chikululupiro, ine nili na zintchito." Nilangize chikululupiro chako cilibe zintchito naine nizakulangiza chikululupiro changa mu zintchito zanga. ¹⁹ Ukululupira kuti kuli Mulungu umozi; uchita bwino. Koma na vimizimu voipa vikululupira ivo, naku njenja. ²⁰ Ufuna kuziba, iwe muntu opusa, kuti chikululupilo chamene chilibe zintchito chilibe pindu? ²¹ Kansi Abrahamu tate watu sana vomelezewe na zintchito pamene eve anapeleka Isaki mwana wake pa guwa? ²² Uwona kuti chikululupiro chake chinasebenzela pamozi na zintchito zake, ndipo kupitila mu zintchito zake chikululupilo chake china kula mofikapo. ²³ Malemba yanakwanilisika yamene yakamba kuti, "Abraamu anakululupila Mulungu, ndipo chamene ichi chinapendewa kuli eve kunkala chilungamo," ndipo anaitaniwa kunkala muzake wa Mulungu. ²⁴ Muona kuti nikupitila muzintchito mwamene muntu amankala oseyewa olungamisiwa, osati muchikululupiro chabe ²⁵ Chimozi-mozi, nanga simwamene Rahabu wachiwere-were anaweluziwa olungama, pamene eve analandila batumiki nakuba pelekeza munjila inangu? ²⁶ Chifukwa mwamene tupi inkalila ilibe moyo ngati ilibe muzimu, chimozi-mozi, chikululupilo chamene chilibe ntchito zolangisa nichakufa.

Chapter 3

¹ Osati bantu bambiliu bankale bopunzisa, abale banga. Tiziba kuti tizalandila chiweluzo chikulu. ² Chifukwa timakangiwa munjila zambili. Ngati muntu ali onse sama lakwa mu mau, uyu nimuntu wofikapo, okwanilisa kulamulila tupi yake yonse. ³ Onani ngati timaika tuntu mu kamwa kama horse kuti yeve yatimvelele, tingakwanise kulamulira ma tupi yabo yonse. ⁴ Onani nama bwato, yangankale niyakulu mutundu bwanji naku yenzewa na chi mpembo chikulu, koma yama yenzewa nakantu kangóno kuli konse kwamene eve oyenza afuna. ⁵ Chimozi-mozi lilimi nikantu kang'ono ka mutupi, koma kama zimvela pavintu vikulu. Onani futi mwamene kamulilo kangóno kama yasha sanga ikulu maningi. ⁶ Lilimi na yeve ni mulilo, chalo chama chimo chamene chinaikiwa pakati pa tupi yatu. Kama ononga mubili onse naku ika pamulilo mayendedwe ya umoyo. Koma nakeve kama ikiwa pamulilo ku gehena. ⁷ Nyama zamutundu onse zamu sanga, tunyoni, na volengewa va mumanzi vima sungiwa komanso vinali kusunguwa na muntu. ⁸ Koma lilimi, kulibe pa bantu wamene amakwanisa kuisamalila. Nichintu chamachimo chosakwanilisa kuchilamulila, chozula na voipa. ⁹ Na eve tima tamanda Ambuye na Atate, komanso naku tembelela bantu, bamene bana pangiwa mukulinganisa Mulungu. ¹⁰ Kuchokela mukamwa kamozi muchoka daliso na tembelelo. Abale banga, ivi vintu visazichitika. ¹¹ Nanga poyambila mumana pamachoka manzi yabwino na voipa? ¹² Nanga mutengo wa mukuyu, abale, uma lenga ma Olivi? Kapena kamutengo ka ma gilepu, mukuyu? Iyayi sichingachitike kuti manzi yamu chele yachose manzi yabwino. ¹³ Nanga nindani wanzelu komafuti womvesesa pakati panu? Mulekeni uyo muntu aonese umoyo wabwino kupitila muvochita vake mukuzichepesa mwanzelu. ¹⁴ Koma ngati ndimwe baukali muvokumbwila nafuti vofuna mumitima zanu, musa zitukumule nakunama boza kushusha vazoona. ¹⁵ Ivi sinzelu zamene zichoka kumwamba. Koma, niza pa chalo, zilibe uzimu, zamizimu zoipa. ¹⁶ Chifukwa pamene papezeka kuzikonda na kukumbwila, pali musokonezo and navonse voipa. ¹⁷ Koma nzelu zamene zichokela kumwamba zilibe koipa, za mutendele, zozichepesa, zozipeleka, zozula na chifundo komafuti zazipaso zabwino, zosapatulula komanso zacho-ona. ¹⁸ Chipaso cha chilungamo chima shangiwa mu mutendere pakati pabaja bamene bama panga mutendere.

Chapter 4

¹ Nanga kushushana naku vutana pakanu kanu kuchoka kuti kansi? Kansi sicvichoka mu kukumbwila kwanu kamene ku menyana mumatupi yanu? ² Mufunisisa, koma simunkala navo. Mumapaya naku kumbwila, koma simukwanilisa kutenga. Mumenyana naku vutana. Simukwanisakunkala navo chifukwa simupempa. ³ Mupempa koma simulandila chifuka simupempa bwino, chifukwa mufuna kuti muchisebenzese pa vofuna vanu. ⁴ Imwe bantu bachigololo! Nanga simuziba kuti kupanga bwenzi nava muziko ni chizondo na Mulungu? Mwa ici, ali ense wamene afuna kunkala muzake wa vamuziko azinkalisa ozondewa na Mulungu. ⁵ Kapena muganizila kuti malemba yakamba mwa chabe kuti, "Muzimu wameme analenga kunkala muli ise niwa kaduka"? ⁶ Koma Mulungu amapeleka chisomo chambili, mwamene malemba yakambila, "Mulungu ama shusha bozitukumula, koma amapeleka chisomo kuli baja bozichepesa." ⁷ Mwa ici, zipelekeni kuli Mulungu. Kanani mudyelekezi, ndipo azataba kuchoka kuli imwe. ⁸ Bwelani pafupi na Mulungu, ndipo na eve azabwela pafupi na imwe. Sambani manja, imwe ochmwa, ndiponso wamyani mitima zanu, imwe bamaganizo yoshushana. ⁹ Mvelani kuipa, nkalani na chisoni, lilani! Lekani kuseka kwanu kunkale chisoni ndiponso chimwemwe chanu chinkale chisoni. ¹⁰ Zichepeseni pa menso ya Ambuye, ndipo azamukwezani. ¹¹ Musankambe wina pa muzake, abale. Muntu wamene akamba pali muzake kapena aweluza mubale wake akamba kushusha lamulo komanso aweluza lamulo. Ngati muweluzi lamulo, sindimwe bokonka lamulo, koma oweluza. ¹² Koma niumozi opasa lamulo komanso oweluza. Eve ndiye wamene akwanisa kupulumusa naku ononga. Nanga iwe ndiwee ndani, iwe wamene uweluza muzako? ¹³ Manje mvela, iwe wamene ukamba kuti, llelo kapena mailo tizaenda kumu zinda uyu, tikankaleko chaka chimozi, tikachite malonda, nakupezako pindu." ¹⁴ Nanga nindani wamene aziba wamene vizachitika mailo, ndiponso umoyo wako nichani? Chifukwa iwe ndiwe mame yamene yaonekela kantawi kang'ono futi naku soba. ¹⁵ Koma, uyenela kukamba kuti, "ngati Ambuye avomelea, tizankala naku chita ivi kapena vija." ¹⁶ Koma onani muzitukumula muma lingo yanu. Konse uku kuzitukumula nichimo. ¹⁷ Mwa ici ali yense wamene aziba kuchita chintu chabwino koma sachichita, kuli eve nichimo.

Chapter 5

¹ Bwelani manje, imwe bolemela, lilani mopunda chifukwa cha mavuto yamene yabwela kuli imwe. ² Chuma chanu chaonongeka, navovala vanu vadyewa na vidoyo. ³ Golide na siliva yanu yaonongeka. Kuonongka kwabo kuzankala kamboni osusha imwe. Chizadya nyama yatupi yanu mona mulilo. Munasunga mozula chuma chanu kusungila masiku yosilizila. ⁴ Onani, malipilo ya wantchito yalila-malipilo yamene munakana kulipila baja bamene banakolola minda zanu, na kulila kwa bokolola kwa fika mu matu ya Ambuye wa makamo. ⁵ Munankala mozimvesa bwino pa ziko na kusangalalisa moyo zanu. Munainisa mitima zanu kulindila siku ya pwando. ⁶ Muna weluza naku paya muntu olungama. Sana ku shusheni. ⁷ Mwa ici nkalani oleza mutima, abale, mpaka kubwela kwa Ambuye. Onani, mulimi ama embekezela vokolola vake vamutengo vochokelela mumunda. Amankala oleza mutima kulindila, mpaka pamene alandila mvula yoyamba na yosilizila. ⁸ Naimwe, chimozo-mozi, nkalani odeka mutima. Limbikisani mitima zanu, chifukwa kubwela kwa Ambuye kuli pafupi. ⁹ Musadaundaule, abale, wina pali muzake, mwakuti musaweluziwe. Onani, eve oweluza aimilila pa chiseko. ¹⁰ Tenganiponi chisanzo, abale, pa kuvutika na kudeka mutima kwa aneneli, bamene bana kamba muzina ya Ambuye. ¹¹ Onani, tima lemekeza baja bana pilila kuti nibo dalisika. Munamvela kulimbikila kwa Yobo, ndipo muziba lingo ya Ambuye, mwamene balili na chikondi komanso ba chifundo. ¹² Pavonse, abale, musalape, kapena kumwamba kapena pansi, kapena kulapa kuli konse. Koma, lekani "kuvomela" kwanu kunkale "kuvomela" na ku "kana" kwanu kunkale "kukana," mwakuti musagwele muchiweluzo. ¹³ Nanga pali aliyense pakati panu wamene avutika? Mulekeni apempele. ¹⁴ Nanga pali wamene ali na chimwemwe? Mulekeni aimbe nyimbo zama tamando. Nanga pali odwala? Mulekeni aitane bakulu bamu pingo, lekani bamupempelele. Lekani bamu zoze na mafuta muzina ya Ambuye. ¹⁵ Pempelo ya chikululupilo izachilisa eve odwala, ndipo Ambuye baza muimya. Ngati anachimwa, Mulungu azamu kululukila. ¹⁶ Mwa ici lapani machimo yanu kuli wina na muzake, ndiponso mupempelelane, mwakuti mu polesewe. Pempeleo ya uja olungama niya mpavu mukusebenza kwake. ¹⁷ Eliya anali muntu monga ise. Anapempela mokululupira kuti mvula isagwee, ndipo mvula si inagwe paziko zaka zitatu na myezi sikisi. ¹⁸ Ndiponso Eliya anapempela kachibili. Kumwamba kunapeleka mvula, na minda inapeleka vipaso vake. ¹⁹ Abale, ngati wina aliyense ataika kucho-onadi, ndiponso winangu amubweza, ²⁰ uja muntu ayenela kuziba kuti aliyense wamene abwezela ochumwa kuchoka mukutaika kwake amupulumusa ku imfa, komanso azavinikila machimo yambili.

1 Peter

Chapter 1

¹ Petulo, wachinto wa Yesu Klisitu, kwa amene siba mutundu wao panthawi iyo, kwa bonse bo sankiwa, kupitila zimene Pontas, Galatia, Kapadosia, Ezhia, na Bitinia. ² Izi nizolingana nazamene anazibilatu Mulungu atate, zimene anapatula mwa muzimu mwa kuvelela motila magari ya Yesu Klisitu. chifundo chinkale naimwa, namutendele wanu upake. ^{3 4 5} mulungu atate nanbuye wa yesu kilisitu adalisike. muchifundo chaka chikulu, anatipasa kubadwa kwanyowani nakulimbikilila naza mene tizapasiwa. izi zopasiwa zinachoka muku uka kwa Yesu Klisitu kuchoka kubakufa. ichi nichazopasiwa zosa onogeka, zilibe madoti, nazamene sizizakasila. ina sungiwiwa iwe kumwamba. indimwe ochingilizwa nanphanvu yamulungu mwa chikulupililo, mwachipulumuso chamene chilipafupi kuonekela munthawi yosiliza. ⁶ Ndimwa okondwela maningi chifukwa chaichi, nangu kuti nichofunikila kuli imwe kuti musavele bwino chifukwa chazovuta zosiyana, ⁷ Ichi nichaku onesela chikulupililo chanu, nicho dula kuchila na golide yeve imaonogeka, pamene bamaiyesa kuika pa mulilo. ichi chima chitika kuyesa chikulupililo chanu kuti chiipezeke mukulemekeza, kupasa ulemelelo, na ulemu pakuonekela kwa yesu klistu. ⁸ Mukalibe kumuonapo, koma mumukonda. Simumuona apa, koma mukhulupilila mwa eve nakukondwela maningi nachikondwelelo chosaneneka chaulemelelo. ⁹ Apa manje mulandila zamene zipezeke muchikulupililo canu, chipulumuso camoyo canu. ma ¹⁰ Profita bana sakila bwino za chipulumuso, zachifundo chamene chizankhala chanu. ¹¹ bana sakila kuti ba ziba nizandani naliti muzimu wa yesu mwabeve unali kukamba kuli beve. izi koma zinachitika pamene anali kubauzilatu zamwa mene yesu analikuyenda kuvutikila nazaulemelelo zokonkapo pambuyo ¹². chinaonesewa kuli beve kuti sibazazipulumusa beka, koma imwe, pamene bana kamba pavintu vame manje viuziwa kuli imwe kuli baja bana lalikila mau yabwino ya mulungu mwamuzimu oyela otumika kuchokela kumwamba-vintu vame ba ngelo benzo funisisa

kuona.¹³ muyenela kuchingiliza nzelu zanu.onani kuti nzelu zanu sizo kolewa.ikani kukulupilila muchifundo kwamene kuza letewa kuli imwe pakuonekela yesu klistu¹⁴ .Monga bana onvelela,osavelela zochita zanu zakudala zamene munali kuchita pamene simunali kuziba.¹⁵ Monga anakuitanani nioyela,nkalani oyela,nkalani oyela muzonse zochita zanu¹⁶ .Pakuti nicholembewa;nkalani oyela,chifukwa ndine oyela¹⁷ .Ndiye pamene muitana kuti atate amene amaweluza osapita kumbali koma kulingana nanchito yamene aliyense agwila,tayani ntawi yaulendo wanu naulemu.¹⁸ muziba kuti simwa golide nasiliva yamene ionongeka yamene munaombolenka nayo kuchoka kuchita vintu mopusa kwamene munapunzinla kwa atate banu¹⁹ .Koma munaomboleka namagazi yodula ya klistu,amene enze monga nkonsa ilibe chimo nangu doti.²⁰ klistu anasankiwa chalo chikalibe kupangiwa,koma aonesewa kuli imwe kutawi ino yosiliza²¹ ,Kupitila muli eve mumukulupilila mulungu,amene ana muusa kuba kufa kwa eve anabapasa ulemelelo kuti chikulupililo chanu nakulimbikila kunkale mwa mulungu.²² Munapanga moyo yanu bwino pakumvelela chazoon²³ .Ichi chinali chachi kondi chapachi bululu,muyenela kukondana kuchokela pansi pamtima.Muna badwa mwa nyowani,osathi nambeu yo onongeka,koma nambeu yamene sionongeka,kupitila mukunkala kwa mau na kusala kwa mau ya mulungu.^{24 25} pakuti ma tupi yonse yali monga mauzu.na mauzu yama yuma,namatepo yamagwa nakuyuma,koma mau yamulungu siyazaka sila.Iyi ndiye nkani yabwino yamene yanaenziwa kuli imwe.

Chapter 2

¹ pavonse fakani kumbali vonse vo ipa, zonse zaboza, za maboza, za kaduka, na zonse zonyoza ² .Monga bana bang'ono, funisisani meleki yamumu zimu wabwino, mwaichi muzakula muchikulupililo ³ .Kapena mwa nvela kuti mulungu niwa mtima wabwino. ⁴ Bwelani kwa eve mwala wa moyo amene anakaniwa nabantu, koma anasankiwa na mulungu alinamtengo odula kwa eve. ⁵ Naimwe muli monga mwala omangika panyumba yau zimu. kuti munkala bo yela bansembe opeleka zensembe za uzimu zovomeleka kwa mulungu kupitila muli yesu klist. ⁶ Mubaibo muli izi "onani, ni ika muzayoni mwala wa paconna, osankika wamutengo odula Ali onse okulupilila eve sazanvesewa nsoni. ⁷ Ulemu niwa imwe manje okulupilila. ⁸ Koma "mwala wamene omanga bana kana wankala osankiwa, uyu wankala mutu wa wapa conna, 'ndipo' unankala mwala ozibuntulamo. Na kugwa" ba gwelapo, kusanvelela mau, yamene yana ikiziwa ku sogolo kwao. ⁹ koma ndimwe osankika ba mulungu, mutundu wosankika, ziko yoyeleseka, bantu bake bamulungu, kuti munene zabwino zochita za mulungu amene anakuchosani kuza mufinzi nakuku ikani odabwisa mo onekela. ¹⁰ kudala simunali bantu, koma manje ndimwe bantu bake mulungu. simwenze munalandila chifundo, koma manje mwa landila chifundo. ¹¹ okondeka, nikuitanani monga balendo nabo endaenda osiya zaku mubili, zamene zima chita ndeo na moyo wanu. ¹² Muyenela ku chita bwino pamene muli paosaniziba, kuti, kapena bakamba kuti munachita vintu zoipa, kutibaone nchitozanu zabwino kuti bayamike mulungu pakubwela kwake. ¹³ Nvelelani ulamulilo onse wabantu ¹⁴ kamba ka mulungu. Nvelelani ma nfumu yolamulila, na onse olamulila, otumika kunzunza ochita zoipa nakuyamikila ochita zabwino. ¹⁵ Pakuti ichi nichifunilo chake mulungu, pakuchita chabwino muzina zokamba zabantu osaziba. ¹⁶ Monga bantu omasuka, osa sebenzesa kumasuka kwanu kuchingiliza zoipa, koma nkalani monga banchinto ba mulungu. Koma ¹⁷ Lemekezani bantu bonse. kondanani pa chibululu chanu. yopani mulungu. Lemekezani Mfumu. ¹⁸ Banchinto "nvelelani mabwana banu naulemu onse. Munkhale ovelela osatichabe mabwana babwino koma naboipa chitani bwino. ¹⁹ Kufunika kuba totela bamene balimbikila nangubapita muzovuta kambako ziba Mulungu. ²⁰ Nanga chifukwa chani munga yamikiwe pamene mwachita chimo koma mwalimbikila? Koma mukachita chabwino koma mwavutisiwa? Ichi nicho lemekeza kwa Mulungu. ²¹ Kamba kaichi munaitanidwa, chifukwa Yesu anakuvutikilani, anachita ichi kuti mukopele muyende njila yake. ²² Sanachitepo chimo, olo zonama kupezeka mukamwa mwake ²³ .Pamene bana muyoza sana bwezemo. Pamene anavutiska, sanaba yofwemo. Koma anazipeleka kwawamene amaweluza bwino. ²⁴ Eve ana nyamula machimo yatu pa mutanda kuti tisaka chiteko chimo, kuti tinkalile kuyeseka. Mwazilonda zake tina polesedwa. ²⁵ Monse imwe mwa nkala muyenda-yenda monga nikosa yotaika, koma manje mwabwezewa kwamulungu endiye okusogolelani moyo.

Chapter 3

¹ Mwaichi' imwe okwatiwa nvelelani ba muna banu. Chitani ichi nangukuti amuna banu samvelela mau, an'nga tembenuke nangu kulibe mau, mukupitila muzochita za bakazi bao. ² Baza ona zochita zao zabwino za ulemu. ³ Asachite nazo onekela kunja: nazibango zovala kumanja za golide na zovala. ⁴ Mumalo mwake lekani zichitike na mtima wonse, naku kongola kwa bwino kwa mu mzimu, yo kongola kwa Mulungu. ⁵ Pakuti azimai oyela anamu lemekeza munjila iyi. Bana limbikila mwa Mulungu kunvelela amuna bao. ⁶ Munjila iyi Sala ananvelela mwamuna wake Aburam naku muitana ambuye, ndimwe bana bake pamene munvelela cha bwino, napa mene simuyopa mavuto. ⁷ Munjila imozi mozi naimwe ba muna mu nkhole nabagazi banu muku nvelana, monga mukazi niofoka. Mukaziba pasa ulemu monga nibamozi ba nchito na mpaso mu umoyo. Chitani ichi kuti ma pempelo yanu ya yankhiwe yasa chingiliziwe. ⁸ Naposiliza, imwe monse, nkalani ba maganizo yamozi, ba chifundo bokondana, ba mitima yabwino. ⁹ Osabwezela choipa pa choipa naku tukwana paku tukwana, osa chita izo pitilizani ku dalisa chifukwa chaichi muna itanidwa, kuti mutenge daliso. ¹⁰ Amene akonda umoyo wabwino nakufuna kuona zabwino asiye kunena nalilime zoipa zama boza. ¹¹ Achoke ku choipa achite chabwino, afunne mtendele aupilikise. ¹² Menso ya Mulungu yaona oyela, namatu yake yanvela zopempa zao. Koma chinso cha Mulungu chimaukila ochita zoipa." ¹³ Ni ndani azakuchitani choipa ngati mukonda zabwino? ¹⁴ Koma ngati muvutika chifukwa chakuyela, ndimwe odalisika. Osayopa zamene ba yopa, osa vutisika. ¹⁵ mumalo mwake, ikani Yesu pakati mu mutima mwanu mo yeleseka. Nkalani oko nzenka ntawi zonse pamene mufunsiwa chifukwa nchani mulimbikila mwa Mulungu. Chitani izi mozichepesa na mwaulemu. ¹⁶ Nkhalani namaganizo yabwino kuti bantu okunenani pa umoyo wanu wabwino ba nvele nsoni pazamene muchita zabwino. ¹⁷ Nicha bwino ngati Mulungu afuna, mu vutike pakuchita chabwino osati choipa. ¹⁸ Klistu naye ana vutika chifukwa chama chimo yatu. Eve oyela anatifela, enze oyela, kuti ati bwelese kwa Mulungu. Ana paiwa kumubili koma anauka kumuzimu. ¹⁹ Mwa muzimu, anapita kulalikila kuba mu ndende. ²⁰ Sibana nvelele pamene Mulungu anaba yembekezela mumasiku yanowa. Mumasiku yopanga chi boti na Mulungu ana pulumusa bantu ban'gono-moyo zili chabe 8. kupita mu manzi. ²¹ Ichi ndiye cho oneselako kubatizika kwanu kwa manzi, kubatiza koku pulumusani manje -siku suka monga kwa doti mumubili, koma cho onesela ganizo yabwino ya Mulungu, kupitila muku ukisidwa kwa mwana wake Yesu Klistu. ²² Yesu ali ku kwanja ya Manja ya Mulungu. Ana yenda ku mwamba. Ba ngelo, bolamulila, nampanvu zikazimuvelela.

Chapter 4

¹ Manje, chifukwa Yesu anavutika mutupi, chitani naimwe chimozi mozi, chifukwa bonse bovutika mutupi ni bomwalila kutupi ² .Paizi, muntu waso, pantawi yonse pamene alimumubili, siba nkhalala kuchita zamene bantu bakonda, koma chamene Mulungu akonda. ³ Pakuti ntawi yabwino inapita yamene Mulungu anapasa osa muziba achiti zamene banali kufuna kuti ba chite kukumbwa, kukonda, kukolewa, kukumbwa kumbwa, nakudyela muziko, nakupempela tumba banayamba tosayenela. ⁴ Aba bantu ni bodabwa pamene baona imwe simukanbako voipa vameba bakamba, bama yambakukamba voipa pali imwe. ⁵ Bayembekeze wamene aza weluza bamoyo naba kufa. ⁶ Ndiye chifukwa mau yana lalikiwa kuli bakufa, nangukuti bana ba weluza kumubili, koma bazankala namoyo kumuzimu. ⁷ Kusila kwa vintu kuli pafupi, munkhale ba maganizo yabwino, nkhalani osakolewa muma ghanizo yanu kamba kama pemphelo. ⁸ Pa vhone munkhale okhondana, chifukwa chikhondi chimachingiliza machimo yambili. ⁹ Munkhale osungana ntawi yonse osadandaula. ¹⁰ Monga ali onse ana landila mpaso, mukazizi sebenzesa ku tandizana. Mukazichita izi monga otumiwa babwino banmpaso zosa lipilisa za Mulungu. ¹¹ Chitani monga bolalikila mau ya Mulungu, pamene wina asebenza siyani asebenze nampanvu zonse zamene Mulungu amupasa. Chitani ichi kuti Mulungu bantu bamulemekeze kupitila muli Yesu Klistu. Ulemu na ulemelelo unkhale kwa Klistu kosasila. Amen. ¹² Bokondeka, osaona monga nichachilendo izi zamene mupitamo kuyesewa mumulilo, osa ona monga nichachilendo. ¹³ Koma ,zioneni monga zamene klist Yesu anapitamo,kondwelani. Kuti futi mukakondwele pamene azabwela ku ulemelelo wake. ¹⁴ Kapena munyozewa kamba ka Klistu Yesu ndimwe odalisika. Chifukwa muzimu wau lemelelo ulipali imwe na muzimu wa Mulungu uli pali imwe. ¹⁵ Koma musa vutike chifukwa chakuti munapaya, kawalala, kuchita zonyansa, ongenela za bene. ¹⁶ Koma kapena wina avutika kamba ka Yesu, lekani asannvele nsoni. Koma siyani alemekeze Mulungu na zina ija. ¹⁷ Chifukwa ntawi ya chiweluzo chiyamba na nyumba ya Mulungu, chikayamba naise, nanga kuli baja ba mene siba nvelela mau ya Mulungu? ¹⁸ Kapena muntu oyela azavutikila kungena kumwamba nanga chizankhala bwanji kuli muntu amene saziba Mulungu? ¹⁹ Lekani bamene bavutika kamba ka Mulungu baike umoyo wao kuo kulupilika anapanga vonse bwino.

Chapter 5

¹ Nilimbikisa ba kulu pakati panu, ine, naine ndine mu kulu muzanu, naine ndine mboni yaku vutika kwa Klistu, naine niza pezekapo pamene aza onesela ulemelelo. ² Mwaicho niku limbikisani, bakulu, sogolelani nkhusa za Mulungu zili pakati panu. Zilanganeni bwino, sikuku kakamizani, koma chifukwa mufuna, kulingana nachifunilo cha Mulungu. Zilondeni, sikamba kandalama, koma mufuna. ³ Osa nkhalu munga ma bwana pa bantu bamene mu sogolela. Koma nkhalani bamene nkhusa ziza onelako. ⁴ Pamene mukulu waba sogoleli aza oneka, muza landila chisote chaulemu. ⁵ Munjila imozi mozi, imwe bana ba nyamata mu yenela, kunvelela ba zimuna bakulu. Bonse imwe valani kuzi chepesa naku tumikilana. Pakuti Mulungu sa funa ozikwezeka. Koma amapasa chifundo ku ozi chepesa, ⁶ Mwaicho mu nkhalu bozi chepesa kuli Mulungu kuti pantawi yake akaku kwe zekeni na kwanja ya mpamvu yake. ⁷ Pelekani zo dandaula zanu kuli Mulungu chifukwa aku samalilani. ⁸ Nkhala ozisungna, nkhalu oyangana. Wamene sunvelana naye satana, alila munga ni nkhalamu, asakila wamene aza ononga. ⁹ Mu ukile. Nkhala olimba mu chikhulupililo. Ziba kuti benango bali muchalo balimbikila ku vutika chimozi mozi. ¹⁰ Muka vutikako mwaka ntawi kangono, Mulungu wachifundo, amene ana ku itanani ku ulemelelo wake wamene siusila muli Klistu. Aku konzani nakuku nkhasikisani, nakuku pasani mpamvu. ¹¹ Kwa Mulungu ku nkhalu kulumulila kosasila. Amen. ¹² Nikumbukila Silvanasi okulupilika, bululu okondewa. Nina ku lembelani pang'ono za eve. Niku limbikisani, nina ku uzani zamene nikamba nicha zoonu chifundo cha Mulungu. Imililani pali ichi. ¹³ Mukazi wamene aliku babiloni, osa nkhiwa pamozi naimwe, akupasani moni. Na maki, mwana mwamuna wanga akupasani moni. ¹⁴ Pasa nani moni mwachi kondi, mutendele unkhale naimwe bonse bamene muli muli Klistu.

2 Peter

Chapter 1

¹ Simon Petulo, kapolo ni mpositoli wa Yesu Khristu kwa onse bamene banalandira chikhulupiliro cholingana na chamene talandira, chikhulupiliro na kuyera kwa mulungu na mpulumusi wathu Yesu Khristu. ² Lekani cisomo na mtendere zinkhale zambiri pa zinthu za Mulungu na Yesu Khristu ambuye athu. ³ Zinthu zonse za mphamvu ya moyo na umulungu zinapasidwa kwa ife pa kuziba Mulungu amene anatitana mwa mphamvu zake. ⁴ Kupitira mwa izi anatipasa malonjezo yambiri yakulu kuti munkhale otengako mbali pa zinthu zabwino, kuti musapezeke mu mabvuto yomwe yali mu ziko chifukwa cha kuzikonda. ⁵ Pa ichi, muyeseko kubweresa mtendere chifukwa cha chikhulupiliro chanu, ubwino wanu kamba ka zamene muziba za Mulungu. ⁶ Pa kuziba kwanu, mufakepo kuzilesa elo pa kuzilesa kwanu mufakepo kukosa elo pa kukosa kwanu mufakepo kuziba Mulungu. ⁷ Pa kuziba Mulungu kwanu mufakepo kukonda ba bululu banu elo pa kukonda banzanu mufakepo chikondi. ⁸ Ngati izi zonse zili mwa inu elo zikula mkati kanu, simuzakangiwa kubala zipaso pa zamene muziba za ambuye Yesu Khristu. ⁹ Koma aliyense amene alibe izi zinthu amaona zamene zili pafupi chabe; alibe menso. Aibala kusukidwa ku machimo yake yakudala. ¹⁰ Manje, ba bululu, muyenera kuyesa kuchita zamushe kuti kuitanidwa na kusankidwa kwanu kusankhale kobvuta. Ngati mwachita izi zinthu, simuzagwa. ¹¹ Ngati mwachita zimenezoniye kuti ufumu wa kumwamba wa ambuye Yesu Khristu uzapasidwa kwa inu. ¹² Koterone nizekhala okonzeka kukukumbusani pa izi zinthu nangu kuti muziba kudala, nangu kuti munakosa kudala mu chikhulupiliro manje. ¹³ Niona ni chinthu chabwino kukukumbusani na kukupasani mphamvu pa izi malinga ngati nili mu tenti. ¹⁴ Chifukwa niziba ati manje-manje nizachosa tenti, munga mwamene Yesu Khristu anionesera. ¹⁵ Nizayesesa kuti mukazikumbuka izi zinthu pamene ine nizayenda. ¹⁶ Chifukwa sitinakonkhe maningi zinthu za boza zamene zinapangidwa pamene tinamuuzani za mphamvu na kuonekera kwa ambuye athu Yesu Khristu. koma tenzeli mboni ya ukulu wake. ¹⁷ Chifukwa analandira kwa Mulungu atate ulemu na ulemelero pamene mau yanaletewa kwa yeve na mphamvu za Mulungu kukamba ati, "uyu ni mwana wanga, okondewa wanga, wamene nikondwera nayeve." ¹⁸ Tinamvera mau aya yamene yanachoka kumwamba, pamene tinali nayeve pa lupiri loyera. ¹⁹ Tili na mau aya ya uneneri yosimikizirika. Muzachita mushe ngati mwamvera. Ili ngati nyale yowala younika mu m'dima kufika kuseneni na nyenyezi ituluka mu mitima yanu. ²⁰ Muziba ichi poyamba, ati palibe uneneri wamene uli na kutantauzila kwa kaena. ²¹ palibe uneneri wamene umabwera pa chifuniro cha munthu. Koma banthu bamene banatengewa na mzimu oyera banamvera kwa Mulungu.

Chapter 2

¹ Aneneri aboza anabwera kwa anthu, naonso aphunzisi aboza azabwera kwa inu. Azaleta zipunziso zaboza, elo bazakana mukulu amene anabagula. Baziletela mabvuto pali beve beka. ² Banthu bambiri bazabakonkha, elo chifukwa cha beve chilungamo chizaonongeka. ³ Chifukwa cha kuzikonda bazapangirapo pindu pali imwe chifukwa cha mau yao yaboza. Chiweruzo chao chizabwera manje-manje; kuonongeka kwao sikugona. ⁴ Chifukwa Mulungu sanaleke angelo bamene banachimwa. Anabapereka kwa Tartarus kuti bankhale mu cheni ya kumidima mpaka pa nthawi ya chiweruzo. komanso, sanalekelele dziko la kudala. ⁵ mu malo mwake anasunga Noah wamene anali oyer mtima, pamozi na benangu asanu ndi awiri, pamene analeta mvula yosasila pa dziko la banthu ochimwa. ⁶ Mulungu anaonongaso Sodom na gomorrah na moto, ngati chisanzo cha chilango chamene chizabwera kusogolo. ⁷ Koma Lot oyer, amene enze anankhala pakati pa banthu ochimwa, Mulungu anamupulumusa. ⁸ Kwa uja munthu osachimwa, amene enze kunkhala pakati pao masiku onse, enzeli kubvutika mu mtima pa zimene anali kuona na kumvera. ⁹ Mulungu amaziba mopulumusila anthu ake kuchoka mu mayesero, na kuziba motengera banthu oipa kuti balandire chilango pa siku la chiweruzo. ¹⁰ Izi zinkhala zoonza kwa baja bamene bapitirira kuchita zinthu zoipa kulingana na zamene thupi lao lifuna nakukana kumvera lamulo. Ndi olimba mtima komanso odzala ni chifuniro. Sayopa kunyoza banthu ozozedwa. ¹¹ Angelo ali ndi mphamvu zambiri, koma sabweresa manyozo ya chiweruzo pa iwo kwa ambuye. ¹² Koma izi nyama zopanda nzeru zinapangiwa kuti zigwidwe mu chionongeko. Saziba chamene atukwana. Muchionongeko ¹³ bazapeza mpaso ya machimo ao. Aona monga kusangalala kwa masana nikwabwino. ni odesedwa na zoipa. Amamva bwino akamachita zinthu zao zoipa pomwe alikudya nanu. ¹⁴ Ali na menso yozula na bakazi ba chiwelewele; sakhutira nao machimo. Amatuntha mitima yofoka kuti yachite zoipa, ndipo mitima yao yanaphunzidwa kukhumbwa vinthu. Ni bana ba tembelero. ¹⁵ Ataya njira yabwino. Anasokera, nasata njira ya Balaam mwana wa Boer, omwe akonda kulandira malipiro ya machimo. ¹⁶ Koma analandira chizuzulo pa zoipa zake. Bulu osakamba koma kukamba mau ya munthu analetsa utsiru wa mneneri. ¹⁷ Anthuwa ali ngati nyenje yopanda madzi. Ali ngati mmakumbi yamene mphepo imayendesa. Mdima olema unasungwa pali beve. ¹⁸ Bakamba na nthota zopanda pindu. Bamanyengelerana banthu na zofuna za thupi lao. Bamanyengelerana banthu bamene bafuna kuthaba bamene bankhala mu zoipa. ¹⁹ Bamalonjeza mutendere kwa beve, koma beve nibakapolo ba zoipa. Chifukwa munthu nikapolo wa vamene vimubvuta. ²⁰ Aliyense wamene apewa chionongeko cha dziko lapansi kusebenzesa chizibiso cha Yesu Ambuye wathu, koma abweleranso ku zoipa, ndiye kuti chothera chinkhala choipa maningi kuchira choyamba. ²¹ Chinakankhala bwino kuti sibanzibe zabwino kuchira kuziba na kubwelerana futi ku zoipa kusiya malamulo yamene yenze banapasiwa. ²² Mwambi uyu niwazoonza pa beve: " galu abwelerana futi ku vamene waluka. Nkhumba yosambika bwino imabwelerana futi ku matika."

Chapter 3

¹ Manje, nilemba kwa inu, okondewa, nkhalata iyi ya chiwiri ngati chikumbuso cha ku maganizo yanu, ² kuti mukumbukire zamene zinakambika kudala naba neneri oyera na lamulo la ambuye Yesu Khristu kupasiwa naba positoli banu. ³ Ziwani izi poyamba, kuti banthu bovuta bazabwera mu masiku yosiliza. Bazakamba voipa na kupitirira kuchita zofuna zao. ⁴ Bazakamba, " ili kuti lonjezo ya kubweraso kwake? kuchoka pamene batate bathu banagona zinthu zonse zili chimozi-mozi, kuchoka pamene chalo chinapangiwa." ⁵ Baibalira dala kuti kumwamba na dziko la pansi zinapangiwa kuchoka ku manzi na manzi, kudala kulingana na malamulo ya Mulungu. ⁶ Nakuti chifukwa cha izi zinthu, dziko la kudala linaonongewa, kuzula na manzi. ⁷ Koma manje dziko liyembekeza chiweruzo cha muliro kulingana na lamulo limozi-mozi. Bachisungira siku la chiweruzo na kuonongeka kwa banthu ochimwa. ⁸ Simuyenera kuibala, okondewa, kuti siku limozi kwa Mulungu ili ngati zaka 1000, elo zaka 1000 zili ngati siku imozi kwa Mulungu. ⁹ Mulungu samachedwa pa malonjezo yake, monga mwamene benangu bangaonere kuchedwa. M'malo mwake niodekha mtima pa inu. Safuna ati umozi wa inu akaonongeke, koma aliyense apange malo ya kuleka zoipa. ¹⁰ Koma, siku la ambuye lizabwera monga kawalala: Dziko lizatha na chongo chachikulu. Zinthu zizapsya na muliro, ndipo dziko na nchito zonse za mkati zizaziwika. ¹¹ Pakuti zinthu zonse zizasila motere, inu muzankhala banthu ba bwanji? Mufunika kunkhala umoyo wabwino wa umulungu. ¹² Mufunika kuyembekeza kubwera kwa siku la Mulungu. Pa siku limenelo, miyamba izaonongewa na muliro, na zonse zizasungunuka kamba ka kupya. ¹³ Koma kulingana na malonjezo yake, tikali kuyembekeza kumwamba kwasopano na dziko lasopano, mwamene banthu babwino bazankhala. ¹⁴ Kotero, okondewa, pakuti muyembekeza izi zinthu, muchite zonse zamene mungakwanise kuti mukapezeke mulibe bvuto pa menso pa Mulungu, muli yeve. ¹⁵ Komanso muone kuchedwa kwa ambuye kunkhala ngati kudekha mtima kwake kukhala cipulumus o, monga momwe m'bale wathu Paulo analembera inu, kulingana na nzeru zamene zinapasidwa kwa yeve. ¹⁶ Paulo akamba pa izi zinthu mu makalata yake yonse, mwamene muli zinthu zobvuta kumvesesa. Mbuli na banthu osankhazikika bamasokoneza zinthu zimenezi, mwamene bamachitira malemba yenangu, kuti bakaonongedwe. ¹⁷ Kotero, okondewa, pakuti muziba izi zinthu, muzichinjirize kuti musasokonezewe na chinyengo cha anthu oipa ndi kutaya chilungamo chanu. ¹⁸ Koma kulani mu cisomo ndi nzeru za ambuye ndi mpulumutsi wathu Yesu Khristu. Ulemelero unkhale kwa yebve lero na nthawi zonse. Amen!

1 John

Chapter 1

¹ Icho camene cenzeko kufumila pachiyambi, camene tinamvwa, camene tinaona na menso yatu, chamene tinapenyeseza, camene tinagwila ndi manja yathu - ichi ndiye ca Mau ya moyo. ² Moyo, unazibisidwa, ndipo tauona, ndipo tiucitila umboni. Tikulalikilani kwa inu za umoyo wosatha, wamene unali ndi Atate, ndipo waziwika kwa ife. ³ Chija camene tinaona ndi kumva ticilankhulanso kwa inu, kuti munkhalenso ndi chiyanjano ndi ife. Chiyanjano cathu cili ndi Atate ndi Mwana, Yesu Kristu. ⁴ Futi tilemba vinthu ivi kuli imwe kuti chimwemwe cathu cinkhale cokwanila. ⁵ Uyu ndiye uthenga wamene tinamva, kucokela kwa iye ndi kulalikidwa kwa inu: Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwayeve mulibiletu mudima. ⁶ Ngati tikamba kuti tili mucigwilizano ndi iye ndipo tuyenda mumudima, tikamba bodza ndipo siticita choonadi. ⁷ Koma ngati tiyenda mukuunika mwamene iye ali kuunika, ndipo mulopa wa Yesu Mwana wake utisukha kumachimo athu. ⁸ Ngati tinena kuti tilibe uchimo, tizinama ife toka, ndipo coonadi sicili mwa ife. ⁹ Koma pamene tivomeleza macimo athu, ali wokhulupilika ndi wolungama kutikhululukila machimo athu ndi kutisambisa ku chosalungama ciliconse. ¹⁰ Ngati tikamba kuti tilibe ucimo, tikumutenga iye kunkhala wa bodza, ndipo mau ake sali muli ife.

Chapter 2

¹ Imwe bana bango'no, nikulembelani izi zinthu kuti musachimwe.koma ngati wina achimwa, tilinaye otipapatila ndi atata, Yesu Kristhu wamene ali oyela. ² Ni muombolo wama chimo yatu, Ndiponso siise teka, Ndiponso wa ziko lonse. ³ Paliichi tiziba kuti timuziba:ngati tasunga malamulo yake. ⁴ Wamene akamba, "Ati ni muziba Mulungu," koma siasunga malamulo yake,ni waboza, na choonadi sichi muli iye. ⁵ koma wamene asunga mau yake,choonadi, ndiye wamane batate ba konda ndi choonadi chake ni chosilizika. paliichi tiziba kuti, timuziba. ⁶ Wamene akamba kuti azankalili muli iye, afunikila kuyenda monga mwame Yesu Kristhu anaendela. ⁷ Okondedwa, sinikulembela malamulo ya sopano kuli iwe, koma niya kudala yamene munali nayo pachiyambi. malamulo yakudala ndiye mau unamvela. ⁸ komanso ni kulembela malamulo yasopano kuli iwe, ndiye ya choonadi muli kristhu, chifukwa mfinzi ilikupita, ndi nyali yachendi ilikuwala kudala. ⁹ Iye wamene anena kuti ali munyali koma azonda mubale wake akali munfinzi namanje. ¹⁰ wamene akonda mubale wake ankallilila mu nyali ndiponso kulibe chamene chingamulenge kuzibuntula. ¹¹ koma wamene azonda mubale wake alimunfinzi ndiponso akalikuyendela munfinzi; ziazi kwamene ayenda, chifukwa nfinzi yaboola menso yake. ¹² Nilembela imwe, bana, chifukwa machimo yanu yakululukidwa chifukwa chazina yake. Nilembela kwainu azitate, chifukwa muziba wamene ili kuchiyambi. ¹³ Nilembela inu amuna achichepele, chifukwa muna gonjesa woyipa. ¹⁴ Nalembela kwainu atate, chifukwa mumuziba uja wamene anali kuchiyambi. Nalembela kwainu amuna achichepele, chifukwa ndimwe olimba, ndipo mau ya Mulungu yankallilila mwa imwe. ndiponso mwagonjesa uja woyipa. ¹⁵ Musakonde ziko angankale zinthu zamenezili muziko. ngati wina wache akonda ziko, ndi chikondi chaatate sichili muli iye. ¹⁶ chifukwa zonse zamene zili muziko_kukumbwila paza muthupi, kukumbwila kwa menso,ndi ntota zaumoyo_siwakuli atate koma niwa kuziko. ¹⁷ ziko ndizo lakalaka zache zili kupita. koma alionse wamene achita chifunilo cha Mulungu azankallilila muyayaya. ¹⁸ Imwe bana bango'no, iyi ni ntawi yosilizila, monga mwamene munamvelela kuti bambili bosusana kristhu babwela.paichi tiziba kuti ni ntawi yosilizila. ¹⁹ Banachokela kuliise , koma sibana chokele mwaise. chifukwa ngati banalikuchokela mwaise, aseme anankhalilila mwaise. koma pamene banaenda, sibalangiza kuchokela kuliise. ²⁰ Koma mulina muzozo kuchokela kuli oyela.ndiponso bonse muziba choonadi. ²¹ sininalembele kwa imwe chifukwa simunazibe choonadi, koma chifukwa muchiziba ichi ndiponso chifukwa kulibe boza yamene ichokela mu choonadi. ²² Ni ndani waboza koma uja wamene akana Yesu kuti ni Kristhu? uja muntthu ni osusana kristhu, chifukwa akana atate ndi mwana. ²³ kulibe wamene aka mwana angankale na tate.Alionse wamene azindikila mwana ndiiyenso alinatate. ²⁴ koma kwaimwe,siyani vamene munasiya kuchiyambi visale muli imwe.ngati vamene munamvela kuchiyambi vasalila mwaimwe, ndiponso muzankhalilila mu mwana ndi atate. ²⁵ Iyi ndiye lonjezo anatipasila: moyo wamuyayaya. ²⁶ Nalemba izi zinthu kamba kabamene bangakukusobeseni. ²⁷ Koma kwaiwe, muzozo wamene unalandila kuchoka kuli iye unkhalilile, ndiponso siufunika wina kukupunzisa. koma mwamene muzozo wake umapunzisa imwe zonse ndiponso ni wachoonadi siwaboza,monga mwamene anakuuzilani nkhalililani muli emve. ²⁸ Manje,imwe bana, nkhalililani muli iye, pakuti akaonekela, tizankhala olimba muthima ndiponso sitizamvesewa manyazi pakubwela kwake. ²⁹ Ngati muziba kuti niolungama, muziba kuti ali onse wamene amachita cholungama niobadwa kuchokela kwaiye.

Chapter 3

¹ Onani chikondi camene Atate anatipasa ife, kuti tiitanidwe ana a Mulungu, ici ndi mwamene tilili. Pa chifukwa ici, dziko lapatsi siitiziba, chifukwa siinamuzibe iye. ² Wokondedwa, manje ndife bana ba Mulungu, ndipo cenze cikalimbe kuonesewa mwamene cizankhalila. Tiziba kuti pamene kristu azaonekela, tizankala ngati iye, chifukwa tizamuona mwemene alili. ³ Aliwonse alina chisimikizo cazakusogolo aika nzelu zake mwaiye ndipo aziyelesa mwamene iye ali woyela. ⁴ Aliwonse wamene apitiliza kucimwa achita vosa vomelekezedwa, cimo nicosa vomelekezedwa. ⁵ Muziba kuti Kristu anaonesedwa kuti achose cimo. Ndipo mwa iye mulibe cimo. ⁶ Kulibe amene akhala mwa iye apitiliza kucimwa, kulibe amene apitiliza kuchimwa anamuona kapena kumuziba iye. ⁷ Bana anga okondedwa, musalole aliwose akusobeseni. wamene achita chilungamo niolungama. ⁸ Monga Kristu niolungama. Amene acita cimo ni wasatana, Chifukwa satana anacimwa kuchoka pachiyambi. Pa chifukwa ici mwana wa Mulungu anaonesedwa, kuti aononge nchito ya satana ⁹ Aliwonse anabadwa mwa Mulungu samachimwa chifukwa mbeu ya Mulungu inkhalilila mwa iye Sangapitilize kuchimwa chifukwa anabadwa kufumila mwa Mulungu. ¹⁰ Mwaichi bana ba Mulungu ndi ana ba satana ba onekela. Aliyense wamene sachita chilungamo sachokela kwa Mulungu, ngakale iye amene sakonde mbale wake. ¹¹ Uyu ndiye uthenga wamene munavela kufumila pachiyambi: kuti tizikondana wina ndi muzake, ¹² osati monga Kaini, amene anacoka kuwoyipa napaya mubale wake. Nanga anamu paila chani? chifukwa nchito zake zinali zoyipa, ndipo mbale wake zinali zachilungamo. ¹³ Osankhala wodabwa, abale anga, ngati ziko ikuzondani. ¹⁴ Tiziba kuti tinapita kucoka ku ifa ndikuyenda kumoyo, chifukwa tikonda abale athu. ¹⁵ Aliyense wamene sakonda akhalila muimfa. Aliyese wamene azonda mbala wake niwakupha. Ndipo muziba ati umoyo wosatha siwu nkhalila mu munthu wakupha. ¹⁶ Mwaichi tiziba chikondi, chifukwa Kristu anataya moyo wake chifukwa ca ise.naise tifunika kutaya moyo wake chifukwa cha abale athu. ¹⁷ koma aliyese ali na kathundu wamuziko, naona mbale wake akufuna nakuvala mutima wake wachifundo kwayeve, Nanga chikondi cha Mulungu chinkhala bwaji mwa iye? ¹⁸ Bana banga okondedwa, tisakonde ndi mau cabe kapena ndililime cabe, koma mukucita ndi mchoonadi. ¹⁹ Ndi mwaici mwamene tiziba kuti tinachokela kuchoonadi, ndipo tisimikiza mitima yasu pamenso pake. ²⁰ Ngati mitima yathu itisusa, Mulungu nimukulu kupambana mitima yathu, Ndipo aziba zithu zonse. ²¹ Wokondedwa, ngati mitima yathu siitisusa, tili ndi chisimikizo kwa Mulungu. ²² Chilichonse camene timpempa tiza landila kuchokela kwa iye, chifukwa tisunga malamulo ndipo tichita zamene zimukondwelesa iye. ²³ iyi ndiye lamulo lake: Kutu tikulupilile muzina ya mwana wake Yesu Kristu ndi kukondana wina ndi muzake, monga mwamene anati phasila malamulo aya. ²⁴ Amene asunga malamulo a Mulungu ankhalilila mwa iye, ndipo Mulungu ankhalilila mwa iye. Mwaichi tiziba kuti akhalilila mwaise, mwa Muzimu wamene iye anatipasa.

Chapter 4

¹ Okondewa,osakululupira muzimu olionse,koma yesani mizimu zonse kuziba ngati ichokela kuli mulungu,cifukwa aneneli aboza agena muziko. ² Pali ichi muzaziba muzimu wa mulungu-muzimu ulionse wamene uzavomela kuti Yesu Kristu anabwela mu munthu achokela kuli mulungu, ³ ndiponso muzimu alionse wamene siuvomela Yesu siuchokela kuli mulungu. Uyu nimuzimu osusana na kristu,wamene munanvela ati ubwela,ndiponso unabwela kudala. ⁴ Munachokela kuli mulungu, imwe bana,ndiponso munabagonjeza,cifukwa wamene alimuli iwe niopambana kuchila wamene alimu ziko. ⁵ Bachokela muziko, navamene bamakamba vichokela muziko,naziko imabanvelela. ⁶ Ise tichokela kuli Mulungu. Wamene aziba Mulungu amatinvelela. Wamene siachokela kuli Mulungu samatinvelela. Pali ichi tizaziba muzimu wachoonadi namu zimu waboza. ⁷ Bokondedwa,tiyeni tikondane,cifukwa chikondi chichokela kuli mulungu.Nabonse bana konda nibobadwa kuli mulungu ndiposo bamuziba mulungu. ⁸ Muntu wamene siamakonda siaziba mulungu,cifukwa mulungu ndiye chikondi. ⁹ Cifukwa chaichi chikondi cha mulungu chinavumbulisiwa pali ise,kuti mulungu anatuma mwana wake eka muziko pakuti tinkale cifukwa cha iye. ¹⁰ Umu mu chikondi,sikuti tinamukonda mulungu,koma anatikonda,ndiponso anatuma mwana wake kunkala otikambilako kuma chimo watu. ¹¹ Bokondedwa,ngati mulungu anatikonda,naise tikondane. ¹² Kulibe anaonapo mulungu. Ngati tikondana mulungu ankala muli ise. Nachikondi chake nichosilizika muli ise. ¹³ Pali ichi tiziba ati tinkalilila muli iye na iye muli ise,chifukwa anatipasako mbali mbali yamuzimu wake. ¹⁴ Ndiponso,tinaona ndikupelekela umboni kuti mulungu anatuma mwana wake kubwela kunkala mupulumusi wa ziko. ¹⁵ Aliyense wamene azavomela ati Yesu nimwana wa mulungu,mulungu azankala mulu iye. ¹⁶ Ndiponso taziba na khukululupira chikondi chamene mulungu alinacho pali ise. Mulungu nichikondi,nawemene ankala muli ichi chikondi ankala muli mulungu,ndiponso mulungu ankala muli iye. ¹⁷ Chifukwa chaichi,ichi chikondi chankala chosililizika pali ise,pakuti tikankale nachisindikizo pasiku yoweluza, monga mwamene alili,ndiye mwamene tilili muziko. ¹⁸ Kulibe manta muchikondi.malo mwa,chikondi chosililizika chimataya manta,chifukwa manta iyendelana na chilango. Koma wamene ayopa sanasilizike mu chikondi. ¹⁹ Timakonda chifukwa mulungu anatikonda pachiyambi. ²⁰ Ngati alionse akamba,"Nikonda Mulungu,"koma siakonda mubale wake, niwaboza.koma wamene siakonda mubale wake, wamene siangakonde Mulungu wamene sianaone. ²¹ Ndiponso iyi ndiye lamulo yamene tilinayo kuchekela kwa iye: Wamene akonda Mulungu afunikanso kukonda mubale wake.

Chapter 5

¹ Alionse wamene akhulupilila kuti Yesu anabadwa kwa Mulungu, ndiponso wamene akonda tate ndiponso akonda mwana wamene anabadwa kwaiye. ² Chifukwa chaichi tiziba kuti tikonda bana bamulungu: ngati takonda ndi kuchita malamulo yamulungu. ³ Ichi ndiye chikondi chamulungu: kuti tisunge malamulo yake. ndimalamulo yake siyolema. ⁴ Aliyense wamene anabadwa kwa Mulungu anagonjesa ZIKO. Ndiponso uku ndiye kupambana kuna gonjesa ziko: mwa chikulupililo chatu. ⁵ Ni ndani wamene angagonjese ziko? Iye wamene akulupilila kuti Yesu ni mwana wa Mulungu. ⁶ Uyu ndiye wamene ana choka ku manzi ndi ku mwazi: Yesu Kristhu. Sianabwele chabe na manzi, koma na manzi ndi mwazi. ⁷ koma kuli zitatu zamene zipeleka umboni: ⁸ Muzimu, manzi ndi mwazi. izi zitatu zimavomekezana. ⁹ Ngati talandila umboni kuchokela kubanthu, umboni wa mulungu ni wa ukulu. koma umboni wa Mulungu ndiye uyu, kuti anapeleka umboni wa mwana wake. ¹⁰ Aliyense wamene akulupilila mwana wa Mulungu alina umboni kwa iye eka. aliyense wamene siakulupilila Mulungu azipanga eka kumkhala waboza, chifukwa sianakulupile umboni wamene mulungu unapasiwa kamba ka mwana wake. ¹¹ Ndi umboni ni uyu: Mulungu anatipasa umoyo wamuyayaya, ndi uyu umoyo uli mu mwana wake. ¹² wamene alina mwana wake alina umoyo. Iye wamene alibe mwana wa Mulungu alibe umoyo. ¹³ Nilembela izi zinthu kuti, kuti muzibe kuti mulina umoyo wamuyayaya_ kuli imwe bamene bakulupilila mu zina la mwana wa Mulungu. ¹⁴ Ndiponso ichi ndiye chizindikilo chamene tili nacho mwa iye, kuti tikamufunsa chilichonse kulinganila na chifuniro chake, ama timvela. ¹⁵ Ndiponso, ngati amatimvela ise_ chilichonse chamene tizamufunsa_ tiziba kuti tapasidwa chamene tamufunsa. ¹⁶ Ngati alionse aona mubale wake achita chimo yamene siipeleka kuimfa, afunika apempele, ndi Mulungu azamupasa umoyo. nikamba oaliaboabo bamene machimo yao siapeleka kuimfa. kuli chimo yamene isanduka ku imfa; sinikamba kuti anga pempele pali icho. ¹⁷ Zonse zamene siziliza ulungamo ni chimo, koma kuli chimo yamene siipelekaku imfa. ¹⁸ Tiziba kuti onse wamene anabadwa kwa Mulungu siamachimwa. koma uyo wamene anabadwa kuchokela kwa Mulungu amamusunga bwino kwaiyo eka, ndiponso uja woipa sianga muononge. ¹⁹ Tiziba kuti tichokela kwa Mulungu, ndiponso tiziba kuti ziko lonse zinkala muzoipa. ²⁰ Koma tiziba kuti mwana wamulungu anabwela, ndiponso anatipasa kumvesesa uyo wamene ilina choonadi. koma, tilinaye wamene alina choonadi, mu mwana wake Yesu kristhu. Mulungu ndiye choonadi ndi moyo wamuyayaya. ²¹ Imwe bana, zichosenikoni kumafano.

2 John

Chapter 1

¹ Kucokela ku mukulu wamupingo kwa mukazi wosankhiwa na bana bake, wamene nikonda muchonadi- ² ndipo sindine neka chifukwa cha choonadi chamene chinasala mwaise ndipo choonadi chizankhalila mwaise muyayaya. ³ Lekani chisomo, chifundo na mutendere zinkale naise kucokela kuli Mulungu Atate nakuchoke kwa Yesu Kristu, mwana wa Atate, muchoonadi namu chikondi. ⁴ Nakondwela maningi kupeza bana banu bana bayenda muchoonadi, monga mwamene tinalandilila malamulo kuchokela kuli Mulungu. ⁵ Apa namupapatilani, mukazi - osati monga nilemba malamulo yasopano, koma amozi tilinaye kuchiyambi - kuti tizikondana. ⁶ Ndiponso ichi ndi chikondi, kuti tiziyenda mumalamulo yakhe. Aya ndiye malamulo, monga mwamene munavelela kuchiyambi, ndipo yenda muli ichi. ⁷ Pakuti bambiri babodza bapita muziko lapansi, ndipo sibazindikila kuti Yesu Kristu anabwela mu tupi. Uyo ndiye wabodza wosusha Kristu. ⁸ Wonesesani pakati panu, kuti musateye zinthu zamene tasebenzela, koma kuti mukalandile mphaso yokwana. ⁹ Aliyense opita pa sogolo ndipo sankhala muchiphunziso cha Kristu alibe Mulungu. Wamene ankhala muchiphunziso, uyu eve alina Atate ndi Mwana. Ngati wina abwela kwanu ¹⁰ ndipo saleta ichi chiphunziso, uyu munthu musamulandile mumanyumba yanu ndipo musamupase moni. ¹¹ Pakuti wamene amupasa moni atengako mbali kuzoipa zake. ¹² Nili na vambili volemba kuli imwe, koma sinifuna kuvilemba na pepala na inki. Motelo, niyembekezela kubwela kwamene uko nikakambe naimwe menso na menso, kuti chimwemwe chanu chinkhale chosilizika. ¹³ Bana ba kalongosi wako osankidwa bakupasa moni.

3 John

Chapter 1

¹ Mkulu wa Gius wamene nikonda muchoonadi. ² Okondedwa nipempela kuti mupambane muvonse nakuti munkale ba thanzi, monga mwamene moyo wanu upita pasogolo. ³ Koma nisangalala maningi pamene abale anabwela kuzapelekela umboni choonadi chanu monga mwamene muyenda muchoonadi. ⁴ Nilibe chimwemwe chopambana ichi, kumvela kuti ana anga mulikuyenda mu choonadi. ⁵ Okondedwa muchita chikhulupiro pamene musebenzela abale nabalendo, ⁶ amene apelekela umboni pachikondi chanu mu chalichi; Chizankhala chabwino ngati muzabatuma paulendo wao munjila yoyenera kwa Mulungu. ⁷ Chifukwa nikamba kazina iyi kuti banayenda osatenga kalikonse kwa Akunja. ⁸ Motero tibalandile kuti tikasebenzele pamozi muchoona. ⁹ Kuli chamene ninalamba ku mpingo koma Diotrefas wamene amafuna kukhala oyamba pakati pao safuna kuti landila. ¹⁰ Motero ngati nabwela nizakumbukila zinchito zake zamene amachita. Mwamene amakambila voipa pali ise, chifukwa sakondwela na mau aya, eve samalandila abale. Amalesa baja bamene afuna kuchita izi ndipo amapisha mu chalichi. ¹¹ Okondedwa musakopele choipa koma chabwino. Wamene achita chabwino aliwa Mulungu. Wamene achita choipa sanaone Mulungu. ¹² Demetrius wamene aliyense amamupelekela umboni na choonadi chamene. Naise tipeleka umboni ndipo muziba kuti umboni wanthu niwazooni. ¹³ Ninali navambili vomulembelani, koma sinifuna kumulembelani na bolo peni, ¹⁴ Koma niyembekezela kumuonani manje manje ndipo tizakambila menso na menso. ¹⁵ Mtendre unkale naimwe. Abale amupasani moni. Mubapase moni abale aliyense na zina yake.

Jude

Chapter 1

¹ Yuda, kapolo ya Yesu Kristu, ndipo mubale wa Yakobo, kwa abo boitanidwa, ndi bokondedwa mwa Tate Mulungu wathu, ndi osungidwa mwa Yesu Kristu: ² Ndipo chifundo, mutendere ndi chikondi vionjezelwepo pa inu. ³ Bokondedwa, pamene nenze kuyeselela na mphavu zanga zonse kuti ndilembe kwa imwe pankaaani ya chipulumuso chathu tonse, chenzo ufunika kuti nikulimbikiseni kuti muvutikile chi khulupiliro chamene chinapasidwa kwise pa thawi imozi na mitima zanu zonse. ⁴ Chifukwa bantu bena babwela kwainu mwakabisila. Aba bantu banakonzekedwa ku kulangiwa. Ndipo nibantu bochimwa bamene beendeka chisomo cha Mulungu watu nochipeleka muuchisilu, ndipo bakana Ambuye Mfumu yatu, Yesu Kristu. ⁵ Apa nifuna kukukumbusani - olo kwenze ntawi ina mwenze bochiziba chonse - kuti Ambuye anapulumsa bantu ba ku Egipito, koma kuchoka paja anabaononga baja bamene sibanakhulupilire. ⁶ Ndipo bangelo bamene sibanasunge mushe udindo wao wa ulamulilo, koma banasiya mhalo yamene benzofunika kunkhalapo - Mulungu anabamanga mumupata wa muyayaya, muminyololo mo fipa, abasungila siku ija ikulu yoweruza. ⁷ Monga Sodoma na Gommora ndi mizinda nzezo bazunguluka, zinachita vigololo ndiponso zichita zina zosayenera kuchitiwa ndi antu. Banabaika chisanzo cha baja bamene banasunzika kuvutika mu moto wosata. ⁸ Manje munjila imozi na imozi aba ba maloto baononga ma tupi yabo. Bamakana ulamulilo, ndipo bamakamba zoipa pali abo ba ulemerele. ⁹ Koma na Mikayeli mukulu wa angelo, pamene enze kusushanya na Satana pa tupi ya Mose sana yese kumuza choyipa yayi. Koma anamuza kuti, "Ambuye akuzuzule!" ¹⁰ Koma aba bantu ba makamba vo kambakamba pa zitu zilizonse zamene sibaziba mushe. Ndipo baziba chabe - monga vinyama vosaganiza viziba muchizibiso - ivi ndiye vinabaononga. ¹¹ Soka kwa eve! Chifukwa banayenda njila ya Kaini, ndipo banizingenesa muku lakwa kwa Balaamu kofuna kudiyelamo. Banaonongekela mu kupanduka kwa Korah. ¹² Aba ndiye bamene bazibisa mumagulu ya ma pwando yachikunja. Ba ma kondyelela kopanda nsoni, bangozidwesa bene beka. Nimakumbi yalimbe manzi, otengewa chabe na mpepo. Ni mitengo zamu ntawi yo panda mvula zilibe vipaso - bokufa kabili, bong'ambika na mizu. ¹³ Ndi mafuunde oyipa pa chimana, bopanga manyazi yabo. Ni nyenyezi zosokera, zimene mudima wakuda unusungiwa masiku osasila. ¹⁴ Enocki, wa nambala seveni kuchoka pa Adam, anapa uneneri pali beve ati, "Onani! Ambuye abwera ndi banthu bambiri makaana na makaana nabo yela bake. ¹⁵ Abwera kupasa chiwerudzo pamunthu onse. Abwera kugojensa bonse bamene bachita nchito zoyipa zamene bachitila mukuyipa kwao, ndipo na mau onse ya ntota yamene aba ba machimo banakamba kwa iye. ¹⁶ Aba bang'ung'uza, ba madandaulo, bamene bakanika zifunilo zao za uchimo. Ndipo ni bozinvela, bamene pakuti vintu vibayendele mushe bekabeka, bama tilimula ba nzao. ¹⁷ Koma, inu bokondedwa, kumbukani mau yamene Ambuye Yesu Kristu anakamba ku mbuyo uku kupitila mu atumwi. ¹⁸ Banakamba kwainu ati, "Mu ntawi yo tera kuzankala banthu boseka chikhulupiliro bamene bazakonika zifunilo zawo za uchimo." ¹⁹ Aba banthu nibopatukisa. Bakonda za muziko, ndipo balibe Muzimu. ²⁰ Koma inu bokondedwa,

zimangeni nhoka muchi khulupirilo chanu cho yela ngako, ndipo mupempele mu Muzimu Oyela. ²¹ Zisungeni mweka mu chikondi cha Mulungu, ndipo yembekezelani chifundo cha Ambuye watu Yesu Kristu chamene chileta umoyo osasila. ²² Nkalani na chifundo kwaibo bamene sibanakhulupirile. Pulumusani bena ndikubachosa mumulilo. ²³ Kuli bena munkhale ba chifundo ndi kuyopa. Muzondenso na zovala zotimbridwa za tupi. ²⁴ Manje kuli iye akwanisa ku khusungungani kuti musazibuntule, ndipo ku pangani kuti muyimilile mu mhalo yake ya ulemerero wake, kulibe kusekewa ndipo nakunkala na chimwemwe chapitilila, ²⁵ kuli Mulungu umozi eka Mupulumusi watu kapitila mwa Yesu Kristu, Mfumu yatu, kunkhale ulemerero, ndi ulamurilo, ndi mphavu, nthawi ikalibo yamba, ndi manje, ndi ntawi zonse. Amen.

Revelation

Chapter 1

¹ Ichi ni chivumbuluso cha Yesu Klistu chamene Mulungu anamu pasa kuti alangize bantchito bake vintu vamene vifunika kuchitika kosa taya ntawi. Anazibisa ichi chintu muku tuma mungelo wake kuli wantchito wake Yohane. ² Yohane anapeleka umboni pa mau ya Mulungu na umboni wa Yesu Kristu, pa vintu vonse vamene anaona eve. ³ Odalisika ni muntu uja wamene abelenga mopunda mau ya uneneli uyu na uja wamene amvela mau ya uneneli uyu na kuikilapo uja wamene akonka vamene vinalembewa mwamene umu, chifukwa ntawi ili pa fupi. ⁴ Yohane, ku mipingo isanu na iwiri ya ku Asiya: Cisomo ni mtendere kucokera kwa iye amene analiko, aliko ndipo azankhalako, ni kwa mizimu isanu na iwiri yamene yankhala pa mpando wa cimfumu, ⁵ na kwa Yesu Khristu, amene ni mboni yokhulupirika, mwana oyamba kucoka pa akufa, ni olamulira mamfumu a dziko lapansi. Kwa iye wamene atikonda ndipo anatiombola ku machimo athu ni magazi yace- ⁶ watipanga kunkhala umfumu, ansembe a Mulungu wake Atate- kwa iye kunkhale ulemelero ni mphamvu kwa nthawi zonse. Amen. ⁷ Onani, azabwera mu makumbi; ndipo diso lililose lizamuona, kuikapo naonse bamene banamulasa. Ziko lonse lizalira chifukwa cha yeve. Inde, Amen. ⁸ "Ndine oyamba na osiliza," akamba ambuye Mulungu, "amene analiko, aliko, elo azankhalako, wa mpamvu zonse." ⁹ Ine, Yohane-m'bale wanu amene agabana na inu zobvuta na kupilira zamene zipezeka mwa Yesu- ninali pa malo ozungulidwa na manzi ya Patmos kamba ka mau ya Mulungu na umboni wa Yesu. ¹⁰ Ninali mu mzimu wa siku la ambuye. Ninamvera kumbuyo kwanga mau okuwa omveka monga lipenga. ¹¹ Yanakamba ati, "lemba zamene uona mu buku, elo uzitume ku mipingo isanu na iwiri- ku Efeso, ku Smyrna, ku Pergamum, ku Thyatira, ku Sardis, ku Philadelphia na ku Laodicea." ¹² Ninapindamuka kuti nione ni mau ya bandani yamene yenze kunikambisa, pamene ninapindamuka ninaona pofaka nyale pagolide pali 7. ¹³ Pakati pa nyale panali wina wamene anaoneka monga mwana wa munthu, anabvala mukanjo utali maningi wamene unafika ku mendo yake na sashi ya golide kuzungulira chifuba chake. ¹⁴ Mutu wake na sisi zinali zoyera monga thonje- zoyera monga matalala, elo menso yake yenze yosweta monga muliro. ¹⁵ Mapazi yake yenze yobeka monga ni bronze, bronze yakuti baifaka pa muliro, elo mau yake yenzomveka monga ni manzi yambiri. ¹⁶ Enze anagwira nyenyezi 7 kumanja yake, na mpeni wamene uchekera mbali zonse unali kuchoka mukamwa mwake. Pamenso pake penzowala monga ni zuba. ¹⁷ Pamene ninamuona, ninagwa pansu pa mendo yake monga munthu wakufa. Anafaka zanja yake pali ine ndipo anakamba ati, "usayope. ndine oyamba na osiliza," ¹⁸ na wamene ankhala na moyo. Ninali wakufa, koma onani, ninkhala wa muyayaya! elo nili na mfungulo ya imfa na hade. ¹⁹ Manje, lemba zamene waona, zamene zilipo manje, na zamene zizachitika kusogolo. ²⁰ Koma pa tanthauzo lobisika la nyenyezi zamene waona mumanja mwanga, na poika nyale pa golide pali 7: Nyenyezi 7 ni angelo 7 a mipingo 7, ndipo poika nyale pali 7 ni mipingo.

Chapter 2

¹ Kwa mngelo wa mpingo wa ku Efeso lemba: aya ndiye mau ya amene anyamula nyale 7 ku zanja la manja na amene ayenda pakati pa zoikapo nyale 7 za golide, ² "niziba zamene wachita na nchito zanu za mphamvu na kupilira mtima kwanu. Niziba ati simunyengelera banthu oipa. Niziba ati munayesa onse amene amaziyesa a positoli, koma si apositoli, elo mwabapeza kuti ni ba boza. ³ Niziba kuti ndinu banthu olimbikira, elo mwabvutika maningi chifukwa cha zina langa, ndipo simunaleme. ⁴ Koma nili chabe na bvuto imozi pali imwe yakuti mwasiya chikondi chamene munali nacho poyamba. ⁵ Kumbukirani sono kwamene mwagwera. Siyani zoipa na kuchita zamene munali kuchita poyamba. Ngati simuleka zoipa, nizabwera kuchosapo poika nyale kuchoka pa malo pamene ilili. ⁶ Koma muli na ichi: simukonda zamene ma Nicolaitans bachita, zamene naine nizonda. ⁷ Lekani wamene ali na matu yakumva amvere zamene mzimu akamba kwa mipingo. Kwa amene apambana, nizamupasa mwai wakudya mu mtengo wa moyo, wamene uli mu paradiso ya Mulungu. ⁸ Kwa mngelo wa mpingo wa ku Smyrna lemba: Aya ni mau ya yeve wamene ni oyamba na osiliza, yeve wamene enze anafa nouka futi: niziba kubvutika kwanu na kusauka kwanu, koma ndimwe olemera. ⁹ Niziba manyozo ya bamene bakamba ati ni ba yuda, koma si bayuda. Nimipingo ya satana. ¹⁰ Musayope zoipa zamene muzapitamo. Onani! satana azaponya benangu ba inu mu ndende kuti mukayesedwe, ndipo muzabvutika kwa masiku 10. Nkhalani okhulupirika mpaka kufa, elo nizakupasani kolona ya moyo. ¹¹ Lekani amene ali na matu ya kumva amvere zamene mzimu ukamba kwa mipingo. Iye amene apambana sazaonongeka na imfa ya chiwiri. ¹² Kwa mngelo wa mpingo wa ku Pergamum lemba: Aya ni mau ya wamene ali na mpeni wonola konse-konse. ¹³ Niziba kwamene munkhala, uko kwamene mpando wa satana upezeka. Koma mupitilira kugwira zina langa. Niziba kuti simunakane chikhulupiliro chanu muli ine, angankhale mu nthawi ya Antipas, mboni yanga, okhulupilika wanga, amene anapaiwa pakati panu, uko kwamene satana ankhalala. ¹⁴ Koma nili na tunthu tung'ono pali imwe: Muli na banthu benangu bamene bagwilirira maningi pa chipunziso cha Balaam, wamene anapunzisa Balak kuika zinthu zoipa pali bana ba Israel, kuti badye chakudya cha vibanda na kunkhala banthu ba chiwelewele. ¹⁵ Chimozi-mozi, muli na benangu bamene banasunga chipunziso cha Nicolaitans. ¹⁶ Siyani zoipa sopano! ngati simuzaleka, nizabwera kwa inu mwamsanga, elo nizachita nkondo na beve na lupanga ili mu kamwa mwanga. ¹⁷ Lekani wamene ali na matu amvere zamene mzimu ukamba ku mipingo. Iye amene apambana, nizamupasa manna yamene yanabisiwa, elo nizamupasa mwala oyera wamene panalembedwa dzina lasopano, dzina lamene palibe winangu amene aziba koma wamene apasidwa chabe. ¹⁸ Kwa mngelo wa mpingo wa ku Thyatira lemba: Aya ni mau ya mwana wa Mulungu, amene ali na menso monga moto na mapazi monga bronze yowala: ¹⁹ "Niziba zamene mwachita: chikondi chanu na chikhulupiliro na zinchito na kulimbikira kwanu. Niziba kuti zamene muchita manje zichira zamene munachita kudala. ²⁰ Koma nili na kanthu aka pa inu: Mumamulekelera mkazi Yezebeli, amene amazikamba ati ni muneneri. chifukwa cha zopunzisa zake asokoneza bambiri bakapolo banga kuti bazichita chiwelewele, nakudya chakudya chamene chapasidwa kwa vibanda. ²¹ Nimamupasa nthawi kuti aleke zoipa, koma safuna kuleka chiwelewele chake. ²² Onani! nizamuponyera pa bedi ya odwala, na onse amene achita naye chigololo bazabvutika maningi, malinga ngati sibaleka zoipa zake. ²³ Nizamupaila bana bake, elo mipingo yonse yazaziba ati ndine amene nimaona maganizo na mitima ya banthu. Nizapasa aliyense wa inu kulingana na zamene muchita. ²⁴ Koma kwa inu benangu baku Thyatira, aliyense amene sazasunga chipunziso ichi, ndipo sibaziba zinthu zobisika zapansi za satana- kwa inu nikamba, 'ine sinizakupasani zinango zolemesa.' ²⁵ Mu njira iliyonse, mufunika kunkhala olimba mpaka nikabwere. ²⁶ Wamene apambana nakuchita zamene nachita mpaka pothera, kwa yeve nizapasa ulamuliro pa maiko onse. ²⁷ Azalamulira maiko na mphamvu, azabapwanya monga mbiya ya dothi. ²⁸ Monga mwamene nalandilira kuli atate, nizamupasaso naine nyenyezi ya m'mawa. ²⁹ Lekani wamene ali na matu amvere zamene mzimu ukamba kwa mipingo.

Chapter 3

¹ "Kwa mngelo wa ku Sardis lemba: Aya ni mau ya wamene asunga mizimu 7 ya Mulungu na nyenyezi 7." Niziba zamene mwachita. Muli na mbiri yakuti muli na moyo, koma ndinu bakufa. ² Ukani na kulimbisa zamene zankhalako, koma zifuna kufa, chifukwa sininapezeke nchito iliyonse yabwino pamaso pa Mulungu wanga. ³ Kumbukirani, sopano, zamene munalandira na kumvera. Gonjerani, na kulapa. Koma ngati simuzauka, nizabwera monga kawalala, elo simuzaziba nthawi yamene nizabwelera kwa inu. ⁴ Koma pali maina yang'ono chabe ya banthu mu Sardis bamene sibanafipise vovala vao. Bazayenda naine, mu zobvala zoyera, chifukwa nioyenera. ⁵ Wamene apambana azapasiwa zobvala zoyera, elo sinizachosa dzina lake mu buku la moyo, ndipo nizakamba za dzina lake kwa atate, na angelo ao. ⁶ Lekani amene ali na matu amvere zamene mzimu akamba ku mipingo. ⁷ Kuli mungelo waku kachissi yaku Filadeofiya lemba: 'Mau ya uja wamene ni oyela nafuti wa zo-ona-wamene agwila mfungulo ya Davide, asecula ndipo kulibe wamene angakome, akoma ndipo kulibe wamene angasegule. ⁸ Niziba wamene munachita. Onani, Naika pameso pako chiseko choseguka ndipo kulibe wamene angachikome. Niziba kuti uli nato tumpavu tung'ono, koma wakonka mau yanga suna kane zina yanga. ⁹ Onani! onse amene achokera ku mpingo wa satana, iwo amene akamba ati ni bayuda koma sibayuda; anama chabe boza. Nizabapanga kuti babwere bagwade pa mapazi yanu, ndipo bazaziba kuti nikukondani. ¹⁰ Chifukwa mwasunga malamulo anga mopilira, naine nizakusungani pa nthawi ya mayeso yamene ibwera padziko lapansi, kuyesa onse amene ankhala pa dziko. ¹¹ Nibwera manje-manje. Sungani bwino zamene muli nazo kuti anthu asalande kolona yanu. ¹² Nizapanga amene alimbikira kunkhala nsandamila ya mnyumba ya Mulungu, ndipo sazatulukamo. Nizalemba dzina la Mulungu pa iye, dzina la mzinda wa Mulungu wanga (Yerusalemu wasopano, wamene uchoka kumwamba kwa Mulungu wanga), na dzina langa lasopano. ¹³ Lekani wamene ali na matu amvere zamene mzimu ukamba ku mipingo. ¹⁴ Kwa mngelo wa mpingo wa ku Laodicea lemba: Aya ni mau ya ma Amen, mboni ya zoona na yodalilika, olamulira chilengedwe cha Mulungu. ¹⁵ Niziba zamene mwachita, kuti sindinu otentha kapena ozizira. Chinakankhala bwino kuti munali otentha kapena ozizira! Tsono, ¹⁶ chifukwa muli pakati-kati- simuli otentha kapena ozizira- nizakulabvulani mkamwa mwanga. ¹⁷ Mukamba kuti, ndinu olemera, nili na zinthu zambiri, ndipo sinifuna kalikonse. Koma simuziba kuti ndinu ochitisa chifundo maningi, osauka, osapenya ni osabvala. ¹⁸ Mvelani zamene nikamba: Gulani kwa ine golide oikidwa mu moto kuti munkhale olemera na zobvala zoyera zowala kuti mubvale musaonese manyazi ya umaliseche wanu, na mankhwala ya m'maso kuti uone bwino. ¹⁹ Nimazuzula aliyense wamene nikonda, ni kuwauza mwamene ayenera kunkhalira. Kotero, cita changu na kutembenuka. ²⁰ Onani! naima pa khomo nigogoda. Ngati wina amvera mau anga na kusegulako, nizaloba mnyumba yake nakudya nayeve, yeve na ine. ²¹ Wamene apambana, nizamupasa mwai onkhala na ine pa mpando wa chimfumu, mwamene ine ninapambana na kunkhala na atate pa mpando wa chimfumu. ²² Lekani wamene ali na matu amvere zamene mzimu ukamba kwa mipingo.

Chapter 4

¹ Pambuyo pa izi zinthu ninayang'ana, ndipo ninaona chiseko choseguka kumwamba. Mau oyamba omwe ninamva omwe yamakamba na ine monga lipenga kukamba ati, "bwera kuno, ndipo nizakuuza zamene zizachitika pambuyo pa izi." ² Pa nthawi imeneyi ninali mu mzimu, ndipo ninaona kunali mpando wa chimfumu ku mwamba, ndipo panali wina onkhalapo. ³ Wamene analipo amaoneka monga jasper na carnelian. Panali utawaleza kuzungulira pa mpando wa mfumu. Utawaleza unaoneka umaoneka monga mwala wa emerald. ⁴ Kuzugulira mpando panaliso mipando 24, ndipo amene anankhala pa mipando imeneyi ni banthu bakulu-bakulu, obvala zobavala zoyera, na ma kolona ya golide ku mutu yao. ⁵ Pa mpando wa chimfumu panachoka moto wa kaleza, kugunda na kung'anima kwa mphenzi. Nyale 7 zimayaka pasogolo pa mpando, nyale zomwe ni mizimu 7 ya Mulungu. ⁶ Pasogolo pa mpando panali msinje wa galasi, monga kirisito. Pakati pa mpando ndi kuzungulira panali zamoyo zinai, zamenso yambiri, kusogolo na kumbuyo. ⁷ Chamoyo choyamba chenze kuoneka monga nkhalamu, cha chiwiri chenze kuoneka monga mwana wa ng'ombe, cha chitatu monga pa menso pa munthu, ndipo cha namba 4 chinali kuoneka monga mbalani youluka. ⁸ Zamoyo zimenez chilichonse chinali na mapiko 6, yozula menso pansi na pamwamba. Usiku na muzuba sivileka kukamba ati, "Oyera, Oyera, Oyera ni Mulungu wa mphamvu zonse amene analiko, aliko, ndipo azankhalako." ⁹ Nthawi zonse pamene za moyo zipereka ulemelero, ulemu na matamando kwa amene ankhala pa mpando wa chimfumu, wamene ankhala kwa muyaya, ¹⁰ akulu 24 amazigwesa pansi kulambira iye amene ankhala pa mpando wa chimfumu. Bamagwada kwa iye amene ankhala muyaya, ndipo amaponya pansi ma kolona yao ku mpando, kukamba kuti, ¹¹ "Ndinu oyenera, ambuye athu na Mulungu wathu, kulandira ulemu, ulemelero ndi mphamvu. Chifukwa munalenga zinthu zonse, ndipo mwa chifuniro chanu, zinankhalako ndipo zinalengewa."

Chapter 5

¹ Ndipo ninaona mumanja mwa iye amene anakhala pa mpando wa chimfumu ku dzanja la manja lake, chi buku cholembewa mbali zonse ziwiri. Inali yosindikiziwa na zosindikizira 7. ² Ninaona mngelo wa mphamvu kukuwa ni mau okweza, "Ndani oyenera kusegula buku na zosindikizira zake?" ³ Palibe aliyense kumwamba, padziko la pansi kapena pansi pa dziko yemwe anali oyenera kusegula buku kapena kuwerenga. ⁴ Ninalira maningi chifukwa panalibe aliyense oyenera kusegula kapena kuwerenga buku. ⁵ Koma m'mozi wa akulu-akulu anati kwa ine, "Usalire. Ona! nkhalamu ya mtundu wa ayuda, muzu wa Davide, wapambana. Akwanisa kusegula buku na kusegula zosindikizira zake." ⁶ Ninaona mwana wa nkhusa kuimilira pakati pa mpando wa chimfumu na zamoyo zinai ndinso pakati pa akulu 24. Anaoneka monga anali ataphedwa. Anali na manyanga 7 na menso 7; Aya ni mizimu 7 ya Mulungu yotumizidwa ku dziko lonse lapansi. ⁷ Anapita ndi kukatenga buku lija ku dzanja la manja la yemwe akhala pa mpando wa chimfumu. ⁸ Pamene mwana wa nkhusa anatenga buku, za moyo zinai ndi akulu 24 anagwa pansi kumulambira. Aliyense anali na mtolilo na mbale yodzala ndi zinthu zonunkhira, yomwe ni ma pemphero ya okhulupilira. ⁹ Anaimba nyimbo ya sopano: Ndinu oyenera kutenga buku ndi kulisegula zosindikizira zake. Chifukwa munaphedwa, ndipo na magari anu munagula anthu a mitundu yonse kwa atate, chilankhulo, mtundu, anthu na maiko. ¹⁰ Munawapanga ufumu, ndi ansembe kutumikira Mulungu wathu, ndipo azakhala pa dziko la pansi." ¹¹ Ndipo ninaona ndi kumva mau ya angelo ambiri kuzungulira mpando wa chimfumu, zamoyo zinai ndi akulu 24. Unyinjira wao unali zikwi ndi zikwi. ¹² Ananena mu mau okweza, "Ndi oyenera mwana wa nkhusa yemwe anaphedwa kulandira mphamvu, ulemelero, nzeru, ulemu na matamando." ¹³ Ninamva cholengedwa chilichonse kumwamba, padziko la pansi, na pansi pa dziko la pansi ni mu manzi- zonse zopezekamo- kukamba ati, "kwa iye okhala pa mpando wa chimfumu na kwa mwana wa nkhusa, kukhale matamando, ulemu, ulemelero ndi mphamvu zolambulira nthawi zonse." ¹⁴ Zamoyo zinai zinati, "Amen!" ndipo akulu anazigwesa pansi ndi kulambira.

Chapter 6

¹ Ninaona pamene mwana wa nkhusa anasegula imozi mwa zosindikizira 7, ndipo ninamva cimozi mwa zamoyo zinai zija kukamba kuti mu mau amene anamveka monga mabingu, "Bwera!" ² Ninaona ndipo panali kavalo oyera. Okwerapo ananyamula uta, ndipo anapasiwa kolona. Anachoka ngati opambana kuti apambane. ³ Pamene mwana wa nkhusa anasegula chosindikizira cha chiwiri, ninamvera chamoyo chachiwiri kukamba ati, "bwera!" ⁴ Ndipo kavalo anatuluka osweta. Wamene anakwerapo anapasidwa mphamvu yochosa mtendere pa dziko la pansi, kuti anthu aphane okha-okha. Okwerapo ameneyu anapasidwa chimpeni chachikulu. ⁵ Pamene mwana wa nkhusa anasegula chizindikiro cha chitatu, ninamvera chamoyo cha chitatu kukamba ati, "bwera!" ninaona kavalo wakuda, ndipo wamene anakwerapo ananyamula muyeso m'manja mwake. ⁶ Ninamvera mau yamene yanamveka kwati niya chimozi mwa zamoyo kukamba ati, "muyeso wa tiligu oguliwa dinari imodzi, ndi miyeso itatu ya balele yogulidwa dinari imozi. Koma osaononga mafuta na vinyo." ⁷ Pamene mwana wa nkhusa anasegula chizindikiro cha namba 4, ninamvera mau ya chamoyo cha chinai kukamba ati, "bwera!" ⁸ ndipo ninaona kavalo ombuwilira. Ndipo okwerapo dzina lake ni imfa, ndipo hade anali kulondola kumbuyo. Anapasidwa mphamvu ya gawo la dziko, kupha na chimpeni, njala na matenda na nyama za musanga za padziko. ⁹ Pamene mwana wa nkhusa anasegula chosindikizira cha namba 5, ninaona pansi pa guwa mizimu ya aja omwe anaphedwa chifukwa cha mau a Mulungu na umboni omwe anali nao. ¹⁰ Analira na mau okweza, "Mpaka liti, olamulira onse, oyera ndi wachoonadi, pomwe muzaweruza omwe ankhala pa dziko la pansi, pomwe muzabwezera magazi athu?" ¹¹ Ndipo aliyense wa iwo anapasidwa mkanjo oyera, ndipo anauzidwa kuti ayembekeze pang'ono mpaka nambala ya akapolo anzao na bale ao ikwane omwe ayenera kuphedwa, monga momwe iwo anaphedwa. ¹² Pamene mwana wa nkhusa anasegula chizindikiro cha namba 6, ninaona ndipo panali chibvomezi champhamvu. Dzuwa inada monga chovala chakutha ndipo mwezi unakhala monga magazi. ¹³ Nyenyezi za kumwamba zinagwa pansi, monga mwamene mtengo wa mkuyu umagwesera zipaso zake zosapya ngati mphepo yakuntha. ¹⁴ Kumwamba kunasoba monga buku lamene alupeteka. Mapiri na zitunda zinachosedwa pa malo ake. ¹⁵ Ndipo mamfumu na anthu olemekwezeka, akulu a asilikali, olemera, amphamvu, ena onse, omasuka ni akapolo, anabisala mu mphanga na mu minyala ya m'mapiri. ¹⁶ Ananena kwa miyala na mapiri, "Tigweleni!" tibiseni ku nkhope ya iye amene ali pa mpando wa chimfumu ni ku mkwiyo wa mwana wa nkhusa. ¹⁷ Chifukwa siku la mphamvu la mkwiyo wao lafika. Ndani azakwanisa kuimilira?"

Chapter 7

¹ Pambuyo pa izi ninaona angelo anai oimilira pa makona anai a dziko, kubweza mwa mphamvu mphepo zinai za dziko kuti mphepo iliyonse isathire pa dziko la pansi, pa nyanja, kapena pa mtengo ulionse. ² Ni naona mngelo wina kuchokera ku m'mawa, amene anali na chizindikiro cha Mulungu wa moyo. Analira mokweza kwa angelo anai aja omwe anapasidwa mphamvu yoononga dziko la pansi na nyanja: ³ "Osaononga dziko la pansi, nyanja ndi mitengo mpaka pamene tizaika zizindikiro pa mphumi pa akapolo a Mulungu." ⁴ Ninamva nambala ya anthu amene anaikidwa zizindikiro: 144,000, omwe anaikidwa chizindikiro kuchoka ku mtundu ulionse wa anthu a Israel: ⁵ 12,000 ochokera mju mtundu wa yuda anaikidwa zizindikiro, 12,000 kuchoka ku mtundu wa Reuben, 12,000 kuchoka ku mtundu wa Gad, ⁶ 12,000 kuchoka ku mtundu Asher, 12,000 kuchoka ku mtundu wa Naphtaly, 12,000 kuchoka ku mtundu wa Manasseh. ⁷ 12,000 kuchoka ku mtundu wa Simeon, 12,000 kuchoka ku mtundu wa L evi, 12,000 kuchoka ku mtundu wa Isaacher, ⁸ 12,000 kuchoka ku mtundu wa Zebulun, 12,000 kuchoka ku mtundu wa Yosefe ndipo 12,000 kuchoka ku mtundu wa Benjamin analandira zizindikiro. ⁹ Pambuyo pa zinthu izi ninaona, ndipo panali anthu ambiri amene palibe angawerenge-kuchoka ku maiko onse, mtundu, anthu na chilankhulo-kuimilira pa mpando wa chimfumu ni mwana wa nkhusa. Anali atamvala zobvala zoyera, ndipo ananyamula nthambi za kanjeza m'manja mwao, ¹⁰ ndipo anali kukamba na mau okweza: "Chipulumuso chichokera kwa Mulungu wathu amene ankhala pa mpando wa chimfumu ni kwa mwana wa nkhusa!" ¹¹ Angelo onse anali oimilira kuzungulira mpando wa chimfumu na kuzungulira akulu komanso zamoyo zinai, ndipo anagwa pansi kuyang'ana nkhoze zao pansi kulambira pa mpando wa chimfumu. Anapembeza Mulungu, ¹² kukamba kuti, "Amen! matamando, ulemelero, nzeru, mayamiko, ulemu, mphamvu, zinkhale kwa Mulungu nthawi zonse! Amen!" ¹³ M'modzi wa akulu ananifunsa ine kuti, "ndani awa, omwe abvala mikanjo yoyera, ndipo achokera kuti?" ¹⁴ Ninakamba nayeve kuti, "bwana, mudziwa" ndipo anati kwa ine, "Awa ndi anthu amene anachoka mu manzunzo yowawa. Awasha mikanjo yao na kuyayeretsa na magazi ya mwana wa nkhusa. ¹⁵ Pa chifukwa ichi, ali pa maso pa mpando wa Mulungu, ndipo amiupembeza usana na usiku mu nyumba yake. Iye wamene ankhala pa mpando wa chimfumu azaika tenti yake pa iwo. ¹⁶ Sazamveranso njala, kapena kumvera ludzu. Dzuwa sizawagwesa, kapena kutenthewa. ¹⁷ Chifukwa mwana wa nkhusa pakati pa mpando azankhala mbusa wao, ndipo azawapereka ku malo a manzi ya moyo, ndipo Mulungu azapukuta misozi mu menso yao."

Chapter 8

¹ Pamene mwana wa nkhusa anasegula chizindikiro cha namba 7, kunali chete ku mwamba kwa theka la ola limozi. ² Ndipo ninaona angelo 7 amene ankhala pa mpando wa chimfumu wa Mulungu, ndipo malipenga 7 yanapasidwa kwa iwo. ³ Mngelo wina anabwera, ananyamula mbale ya golide ya zonunkhirisa, kuimilira pa guwa la zonunkhirisa. Zonunkhirisa zambiri zinapasidwa kwa iye kuti apereke pamozi na mapemphero ya okhulupilira pa guwa la zonunkhirisa pa mpando wa chimfumu. ⁴ Utsi wa zonunkhirisa, na mapemphero ya okhulupirira, yanafikira ku mpando wa Mulungu kuchoka ku manja ya mngelo. ⁵ Mngelo anatenga mbale ya zonunkhira na kuikamo moto wa pa guwa. Ndipo anaiponya pansi pa dziko la pansi, ndipo panali phokoso la kaleza, kugunda na kung'anipa kwa mphenzi, na chibvomezi. ⁶ Angelo 7 omwe anali na malipenga anakonzeka kuti alize. ⁷ Mngelo oyamba analiza lipenga lake, ndipo panali mvula ya mphepo, moto yosakaniza na magari. Inaponyedwa pa dziko la pansi kwakuti gawo lina linatenthedwa, gawo la mitengo inapya, ndi udzu onse obiliwira unapya. ⁸ Mngelo wa chiwiri analiza lipenga lake, ndipo chinthu china chachikulu monga phiri chinaponyedwa mnyanja. Gawo lina la manzi inankhala magari, ⁹ zina mwa nyama za m'manzi zinafa, ndipo ma bwato ambiri anaonongeka. ¹⁰ Mngelo wachitatu analiza lipenga lake, ndipo nyenyezi yaikulu inagwa kuchoka ku mwamba, yoyaka monga tochi, pa gawo lalikulu la misinje na nyenje za madzi. ¹¹ Dzina la nyenyezi ni chobaba. Ndipo madzi yanankhala yobaba, ndipo anthu ambiri anafa chifukwa cha manzi yobaba. ¹² Mngelo wa chinai analiza lipenga lake, ndipo gawo lina la dzuwa linakanthiwa, ndi gawo lina la mwezi na gawo lina la nyenyezi. Sono magawo ambiri anadesedwa; gawo lina la siku na gawo lina la usiku linalibe kuwala. ¹³ Ninaona, ndipo ninamva mphungu yomwe imauluka pakati pa mitambo, kuitana na mau yokweza, "tsoka, tsoka, tsoka, kwa amene ankhala pa dziko la pansi, chifukwa cha malipenga omwe asalira kuti alizidwe na angelo atatu."

Chapter 9

¹ Ndipo mngelo wa cisanu analiza lipenga yake. Ninaona nyenyezi kumwamba yamene inagwa pa dziko la pansi. Nyenyezi inapasiwa makiyi yosegulira mugodi opanda kolekezera. ² Inasegula khomo la mugodi opanda kolekezera, ndipo panachoka utsi monga uchoka pa muliro waukulu. Dzuwa na mphepo zinadesedwa chifukwa cha utsi ochokera ku mugodi wamene uyu. ³ Kuchoka mu utsi dzombe unabwera pa dziko la pansi, ndipo inapasidwa mphamvu monga za kaliza pa dziko la pansi. ⁴ Yanaenziwa kuti yasaononge mitengo kapena udzu pa dziko, koma chabe anthu amene alibe chizindikiro cha Mulungu pa mphumi pao. ⁵ Sibanapasidwe mphamvu zakupha anthu, koma kuwavutisa chabe kwa miyezi isanu. Ululu wake unali monga wa kaliza ngati waluma munthu. ⁶ Masiku ameneo anthu azafuna imfa, koma osaipeza. Azafuna maningi kuti afe, koma imfa izathaba. ⁷ Dzombe inaoneka monga kavalo okonzekera nkhondo. Pa mitu zao panali makolona agolide, ndipo nkhope zao zinali monga za munthu. ⁸ Anali na sisi monga mkazi, ndipo meno yanali monga ya nkhalamu. ⁹ Yanali na vobisa pa chifuwa monga va nsimbi, ndipo chongo chao chinali monga cha akavalo ambiri opita ku nkhondo. ¹⁰ Yanali na michila yolumila monga ya kaliza; ku michila yanali na mphamvu yoluma anthu kwa miyezi isanu. ¹¹ Anali na wina monga mfumu pa iwo mngelo wa ku mugodi opanda kolekezera. Dzina lake mu chi heberi anali Abaddon, ndipo mu chi greek anali na dzina lakuti Apollyon. ¹² Soka loyamba lapita. Onani! pambuyo pa izi pali zilango zina zomwe zibwera. ¹³ Mngelo wa namba 6 analiza lipenga lake, ndipo ninamva mau ochokera mu nyanga ya pa guwa la golide yomwe ipezeka kwa Mulungu. ¹⁴ Liu linanena na mngelo wa nambala 6 yemwe anali na lipenga, "masula angelo anai omwe niomangiwa pa msinje waukulu wa Euphrates." ¹⁵ Angelo anai omwe anakonzedwera nthawi imenei, siku limeneli, mwezi umeneo na chaka chimenechi, anamasulidwa kuti aphe gawo lina la anthu. ¹⁶ Nambala ya anthu omwe anali pa msana wa akavalo ianali 200,000,000. Ninamva nambala yao. ¹⁷ Umu ni mwamene ninaonera akavalo mu masomphenya yanga na iwo okwerapo. Zovala pa zifuwa zao zinali zofilira, zooneka bulumu ni zachikasu. Mitu ya akavalo imaoneka monga mitu ya nkhalamu, ndipo mkamwa mwao mumatuluka moto, utsi, na sufule. ¹⁸ Gawo lalikulu la anthu anafa chifukwa cha zilango zitatu zimenezi: Moto, utsi na sufule zomwe zinachoka mukamwa mwao. ¹⁹ Pakuti mphamvu ya akavalo inali mkamwa mwao na ku muchila kwao- chifukwa michila yao inali ngati njoka, ndipo inali na mitu yamene inali kupwetekera anthu. ²⁰ Anthu ena onse, aja amene sanaphewe na zilango zimenezi, sanalape zoipa zamene anachita, kapena kuleka kupembeza ziwanda na mafano ya golide, siliva, bronze, minyala, na mitengo-zinthu zomwe sizipenya, kumva kapena kuyenda. ²¹ Sanalapenso pa kupha kwao, matsenga yao, chiwelewele chao kapena ncito zao za kuba.

Chapter 10

¹ Pamene apo ninaona m'ngelo wina wamphamvu aseluka kucokela ku mwamba. Anavimbiwa na mukumbi, panali futi na uta wa leza pa mwamba pa mutu wake. Cinso cake cinali ngati zuba na mapazi yake yenze monga vipilala va mulilo. ² Anali naka buku kakang'ono mu manja yake yamene yinali yosegula, na kuika kwendo la ku kwanja la manja pa cimumana na yakumanzele pa mtunda. ³ Pamene apo anapunda namau yopundisa monga ku uluma kwa mkango. Pamene anapunda, zo gunda 7 vinakamba nakuuluma kwake. ⁴ Pamene vogunda 7 vinakamba, nenze pafupi na kulemba, koma ninamvela mau kucokela ku mwamba yakunena, "Sunga nkama ya vimene vogunda 7 vanena. Usavilembe." ⁵ pamene apo mngelo amene nenze naona kuimilila pa mmana na pa calo, ananyamula kwanja lake lamanja ku mwamba. ⁶ Analumbila pa yeve ankala na moyo nthawi yonse, amene anapanga mumwamba na vonse vili mwa mene umo, calo na vonse vili mwa mene, na cimumana na vonse vili mwamene, na mngelo anakamba, "Sikuzankhala futi kucedwa. ⁷ Koma pa siku yamene mngelo wa 7 ali pafupi na kuliza mtolilo, pamene apo codadwisa ca Mulungu cizakwanilisika, monga mwamene ananena ku ba nchito bake maporofita." ⁸ Mau ninamvera kucokela ku mwamba yanalankhulanso kuli ine: "Pita, tenga buku losegula imene ili mu kwanja ya mngelo woimilila pa mumana na pa ziko." ⁹ Pamene apo ninayenda ku mungelo nakumuza kuti anipase ka buku kakang'ono. Anakamba na ine, "Tenga buku na kudy. Izapanga mmala mwako ku baba, koma mkamwa mwako izankala yonzuna ngati uci." ¹⁰ Nina tenga kabuku kakang'ono kucoka ku manja a mngelo na kudy. Inali yonzuna monga uci mukamwa mwanga, nitasiliza kudy, mumala mwanga munababa. ¹¹ Pamene apo wina anakamba na ine, ukambenso za anthu ambili, mitundu, malilime na mamfumu."

Chapter 11

¹ Nteete ina pasiwa kuli ine kuti ni isebenzese monga mutengo opimila. Ni nauziwa "Ima upime tempele ya Mulungu na luwa, na bamene ba pempelelamo. ² Koma usapime lubanza panja pa tempele, chifukwa yapasiwa ku ochimwa. Bazadya-dyaka muzinda oyera kufikila myezi 42. ³ Niza pasa mboni zanga zibili ulamililo kuti bachite uneneri kokwanila masiku 1, 260, bovalikiwa mu masaka." ⁴ Aba bamboni ni vimutengo vama olive vibili na ma tebulu yofakapo nyali yabili yamene yaimilila pamenso pa Ambuye wa ziko. ⁵ Ngati kuli asanka kuvi ipisa, mulilo uchoka mukamwa mwao naku ononga badani bao. Aliyense wamene afuna kubapaisa apayiwe munjila iyi. ⁶ Aba bamboni bali na ulamililo kuvala ku mwamba kuti mvula isagwe mu ntawi yamene bazankala ba nenera. Bali na mpavu zo sandula manzi kunkala magari nakuleta mavuto yali yonse pa chalo pali ponse pamene bafunila. ⁷ Bakasiliza umboni wao, chirombo chochoka mu mugodi wamene susila chiza chita nabo nkondo. Chizagonjesa na ku bapaya. ⁸ Matupi yabo yaza gona mu njila za muzinda ukulu (wamene uitaniwa mumuzimu Sodama na Egipto) kwamene Ambuye babo bana pachikiwa. ⁹ Pama siku yatatu na siku yosa kwanila benangu kuchokaku bantu bonse, mitundo yonse, na ma ziko yonse bazayangana matupi yabo. Sibaza vomelesa kuti yafakiwe mu manda. ¹⁰ Bamene bankala pa ziko ya pansi baza kondwela pali yeve naku sangalala. Baza pasana na mpaso chifukwa aba baneneri babili bana vutisa bantu benzo nkala pa ziko. ¹¹ Koma pakapita ma siku yatatu na siku yosa kwanila mpepo ya moyo yochoka kuli Mulungu izabangena, ndipo baza imilala pa mendo yabo. Kuyopa kukulu kuzagwera bonse baza baona. ¹² Ndipo bazamvela liu ikulu kuchoka ku mwamba kubauza, "Bwera pamwamba pano!" Ndipo baza yenda kumwamba mu makumbi, pamene badani babo ba yanganila. ¹³ Pa ntawi ija kunzankala chivomezi, ndipo imozi ya magawo kumi ya muzinda izagwa. Bantu bali 7, 000 baza paiwa mu chivomezi, ndipo bopulumuka baza yopa naku pasa ulemelero kuli Mulungu waku mwamba. ¹⁴ Soka ya chibili yachoka. Ona! soka ya chitatu ibwela mwamu sanga. ¹⁵ Ndipo mungelo wa chisano na vibili analiza lipenga, ndipo ma liu yakulu yanakamba kumwamba, "Umfumu wapa ziko ya pansi wankala ufumu wa Mbuye watu na Kristu wake. Azalamulila muyayaya. ¹⁶ Ndiponso bakulu bali 24 benze nkale pa mipando yabo ya ufumu pamenso pa Mulungu bana gona pansi na nkope zabo zoyangana pansi. Bana mu lambila Mulungu. ¹⁷ Banati, "Tikuyamikani Ambuye Mulungu Mulamilili wa bonse, wamene aliko, wamene enzeliko, ndipo wamene ali kubwela. ¹⁸ Ma ziko yana kalipa, koma ukali wanu wabwela. Ntawi yabwela kuti bakufa ba weluziwe ndipo kuti imwe mu lambule ba tumiki banu baneneli, baja bokulupilila, na baja bana yopa zina yanu, bonse bang'ono na bakulu. Ndipo ntawi yafika kuti imwe muononge baja bango ononga ziko. ¹⁹ Ndipo tempele ya Mulungu ku mwamba ina seguliwa, ndipo kasa ya chipangano chake inaonekela mu tempele yake. Kwenze tuleza, kufuula, magungu, chikukumo na mvula ya myala.

Chapter 12

¹ Cholangiza chikulu chinaonekela kumwamba: mukazi anavaliikiwa zuba, na mwezi unali pansi pa mendo yake komanso chisote cha ufumu chinali na nyenyezi twelve pamutu pake. ² Anali na pakati, komanso anali kulila na kubaba kofuna ku beleka, nakubaba kwa muzimai wa pakati. ³ Kunkopa kunali cholangiza chinangu chamene china onekela kumwamba: Onani! Kunali chilombo chikulu cha red chamene chinali na mitu seven na nsengo zili kumi, komanso kunali visoti va ufumu vinali seven pa mitu pake. ⁴ Muchila wake una pyanga nyenyezi mumwamba naku yaponya pansi pa ziko. Chilombo ichi chinaimilila pamene panali muzimai wamene anali kuyembekezela kubeleka, mwakuti akabeleka, chidye mwana uja. ⁵ Anabeleka mwana, mwana mwamuna, wamene aza lamulila ma iko yonse na ndodo ya nsimbi. Mwana wake anapokewa kuchoka kuli Mulungu kumuchosako ku mpando wake wa chifumu, ⁶ ndipo mukazi uja anataba ku yenda mu chipululu, kwamene Mulungu ana mukonzela malo yake, mwakuti asalililiwe masiku yokwanila 1,260. ⁷ Manje kunali nkondo ku mwamba. Mika na ba ngelo bake banamenyana na chilombo, chilombo na bangeli bake banamenyana nabo nkondo. ⁸ Koma chilombo sichinali na mpavu zakuti chi gonjese. Chifukwa cha ichi kunalibe malo kumwamba yake na bangelo bake. ⁹ Chilombo chikulu-chija chi njoka chakudala choitaniwa kuti mdyelekezi kapena kuti Satana, wamene anama ziko yonse-chinaponyewa pa ziko, na bangelo bake banataiwila pamozi na eve. ¹⁰ Ninamvela liu ikulu kumwamba: "Manje chafika chipulumuso na mpavu na ufumu wa Mulungu, na ulamulilo wa Kristu wake. Chifukwa eve onamizila babale batu aponyewa pansi, wamene anali kubanamizila pamenso pa Mulungu watu muzuba na usiku. ¹¹ Banamugonjesa kupitila mu magari ya Nkhosa na mau ya umboni wao, chifukwa sibanakonde myoyo zabo kufikila mpaka imfa. ¹² Chifukwa cha ichi kondwelani, imwe mwamba na bonse bamene mulimo! Koma soka ku ziko yapansi na nyanja, chifukwa mdyelekezi agwela pansi pamene imwe mulili! Eve azula na ukali oipisisa chifukwa ali na ntawi ingono! ¹³ Pamene chilombo china zindikila kuti chinataiwa pansi, chinapilikisha mukazi wamene anabeleka mwana mwamuna uja. ¹⁴ Koma mukazi anapasiwa mapepe yabili ya chimbaleme chikulu mwakuti atabile kumalo yamene yanakonzewa kunkala yake muchipululu. Aya yanali malo yamene azasalililiwa, kwa ka ntawi, ntawi, na gawo imozi ya pakati ya ntawi-kuchoka pamalo pa chinjoka. ¹⁵ Chinjoka chinatila manzi kuchoka mukamwa mwake monga mumana, mwakuti yaja manzi yamutenge uja mukazi. ¹⁶ Koma ziko inamutandiza mukazi. Ziko ina segula kamwa kake na kumwa manzi ya mumana yamene chinjoka chinali kuchosa mukamwa mwake. ¹⁷ Manje chinjoka china kalipa na mukazi uja naku yenda kuachaya nkonda na bonse ba mubadwe wake, baja bamene bakonka malamulo ya Mulungu na kugwililila umboni wa Yesu. ¹⁸ Chinjoka chija chinaimilila pa doti yapa mbali pa manzi.

Chapter 13

¹ Ndipo ninaona chilombo chamene chinali kuchoka mu manzi. Chinali na nsengo zili ten na mitu zili seven. Pa nseongo zake panali tusote twa chifumu tunali kumi, pa mutu uli onse panali zina yonyozela. ² Ichi chilombo chamene ninaona chinali monga Lepad. Mendo yake yanali monga mendo ya beya, kamwa kake kanali monga kamwa ka nkalamu. Chilombo ichi chinachipasa mpavu nzake, mupando wake, na mpavu zolamulila. ³ Mutu umozi wa ichi chilombo unali na chilonda cha imfa, koma chija chilonda chinapolesewa. Ziko yonse inadabwa pamene inali kukonka chilombo. ⁴ Bana pembeza chinjoka chija, chifukwa chinapasa mpavu zake chilombo. Bana pembeza chilombo, nacheve, nakukamba kuti, "Nanga nindani wamene angalingane na chilombo?" nanga nindani wamene angachayane na cheve?" ⁵ Chilombo chinapasiwa kamwa kamene kanali kukamba mau yozitukumula na manyozo. Chinavomelesewa kusebenzesa mpavu ntawi yokwanila myezi kumi na zibili. ⁶ Chilombo chinasegula kamwa kukamba mau onyozela Mulungu-kunyoza zina yake, malo yamene ankalamo, na bonse bamene bali ku ziko yaku mwamba. ⁷ Chilombo chinavomelesewa kuchita nkondo na bantu boyela ba Mulungu na ku bagonjesa. Kuikilapo, mpavu inapasiwa kulicheve pa m'tundu uyli onse, bantu, chikambidwe, na ma ziko. ⁸ Bonse bamene bankala pa ziko yapansi bazachipembeza, ali yense wamene zina yake sinalembewe, kuchokela ku chilengedwe cha ziko, mu Buku ya moyo, yamne niya Mwana wa Nkhosa wamene ana paiwa. ⁹ Ngati aliyense ali na kwatu, mulekeni amvele. ¹⁰ Ngati aliyense aenela kutengewa ukapolo, ku ukapolo aza enda. Ngati ali yense ayenela kupaiwa na mupeni, na mupeni azapaiwa. Uku nikuitaniwa kuti mupilire molimbikila ma chikulupiliro kwa bantu boyela ba Mulungu. ¹¹ Nina ona chilombo china chichokela pa ziko yapansi. Chinali na nsengo zibili monga ka mwana ka nkhusa, chinali kukamba monga chilombo. ¹² China sebenzesa mpavu za chilombo choyamba mumalo mwake, chinalenga ziko yapansi na bonse bamene bankalamo kuti bapembeze chilombo choyamba-chamene chilonda chake chinapolesewa. ¹³ China chita vintu vodabwisa vampavu. Chinalenga mulilo kuti uchoke kumwamba pamenso pabantu bonse. ¹⁴ Kupitila mu volangizila vamene anapasiwa kuimililako chilombo, ananama bonse bamene bankala pa ziko yapansi, kubauza kuti baike chifano cholemekeza chilombo chija-chamene chi lengewa chilonda na lupanga, koma sichinafe. ¹⁵ Anavomelezewa kupasa moyo ku chifanikizo cha chilombo mwakuti chifanikizo chija chikazikwanisa kukamba na kulenga bonse bamene banakana kupembeza chilombo kuti bapaiwe. ¹⁶ China kakamiza bantu bonse, bamene sibochuka nabaja bochuka, bolemela nabaja bosauka, bomasuka na bakapolo, kulandila chidindo pa zanja yamanja yaku manja kapena pa mpumi. ¹⁷ Chinali chovuta kuti muntu aliyense agulise kapena kugula chintu koma ngati anali nacho chidindo cha chilombo, kukamba kuti, numero yamene iimililako zina yake. ¹⁸ Ichi chifunika nzelu. Ngati muntu aliyense ali na nzelu, mulekeni apendele numelo ya chilombo. Chifukwa ni numelo ya muntu. Numelo yake ni

666.

Chapter 14

¹ Ninaona na kuona mwana wa nkhusa oimilira pa phiri la Zion. Anali na anthu 144,000 amene anali na zina lake na zina la Atate ake yolembewa pa mphumi zao. ² Ninamvera mau ochokera kumwamba omveka monga manzi yambiri na kugunda kwa mphamvu. Mau omwe ninamvera yanali monga anthu oliza mitoliro. ³ Anaimba nyimbo zasopano pamaso pa Mulungu, zamoyo zinai na akulu. Kunalibe wina opunzira nyimbo imeneyi koma chabe aja 144,000 omwe anaguliwa pa dziko la pansi. ⁴ Aba nibaja bamene sanazidese na akazi, cifukwa anazisunga ku chiwelewele. Niyaba amene alondola mwana wa nkhusa kulikonse kwamene ayenda. Awa anaguliwa kuchoka pa anthu ngati ana oyamba a Mulungu ni mwana wa nkhusa. ⁵ Palibe boza yamene inapezeka mkamwa mwao; niopanda chifukwa. ⁶ Ninaona mngelo wina akuuluka mu mwamba, amene anali na uthenga wa moyo ouza anthu onkhala pa ziko la pansi-ku maiko onse, mitundu yonse, chilankhulo na anthu. ⁷ Anaitana na mau a mphamvu, "yopani Mulungu na kumupasa ulemelero. Chifukwa nthawi ya chiweruzo chake chafika. Mulambileni, wamene anapanga kumwamba, dziko la pansi, nyanja, na nyenje za manzi." ⁸ Mngelo wina-mngelo wachiwiri- anasatira kukamba kuti, "Wagwa, wagwa Babylon wamphamvu, wamene anauza anthu onse kuti amwe vinyo wa zilakolako zake za chiwelewele." ⁹ Mngelo wina-mngelo wachitatu- anawalondola kukamba ati na mau okuwa, "ngati wina apembeza chilombo na chifano chake, na kupasiwa namba pa mphumi kapena pa zanja lake, ¹⁰ azamwa vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, vinyo wamene waikiwa opanda kutirako manzi mu cup ya kukalipa kwake. Munthu amene azamwa azabvutika na muliro na sufule pamenso pa angelo na mwana wa nkhusa." ¹¹ Utsi wa kunzunzika kwao upitilira ku mwamba nthawi zonse, ndipo sapumula usana na usiku-awa opembeza chilombo na fano lake, na aliyese amene analandira chizindikiro cha zina lake. ¹² Apa pali kufunika kupilira kwa iwo amene ni oyera, amene akonkha malamulo ya Mulungu na chikhulupiliro mwa Yesu." ¹³ Ninamva mau kuchoka ku mwamba kukamba ati, "Lemba izi: Odala ni anthu amene anafa mwa ambuye." "Inde," ukamba mzimu, "kuti akapumule ku zolemesa zao, chifukwa nthawi zao zizabalondola." ¹⁴ Ninayangana, ndipo panali makumbi yoyera. Ndipo onkhala pa makumbi anali ngati mwana wa munthu. Anali na kolona ya golide pa mutu pake na chikwakwa chonola ku manja yake. ¹⁵ Ndipo mngelo wina anatuluka mu nyumba ya Mulungu ndipo anaitana na mau okweza kuitana uja amene ali pa makumbi: "Tenga chikwakwa chako elo uyambe kujuba. Chifukwa nthawi yojuba yakwana, cifukwa zokolola pa ziko zapya." ¹⁶ Ndipo wamene anali pa makumbi anayamba kuyendesa chikwakwa pa ziko, ndipo ziko inakololewa. ¹⁷ Mngelo wina anatuluka ku mwamba mu nyumba ya Mulungu; nayeve anali na chikwakwa. ¹⁸ Mngelo winanso anatuluka kuchoka pa guwa la zonunkhirisa, amene anali na ulamuliro pa muliro. Anaitana na mphamvu uja amene anali na chikwakwa chonola, "Tenga chikwakwa chako na kuika pamozi zidunswa za mpesa m'minda ya ziko, chifukwa mpesa wake wanya." ¹⁹ Mngelo anayendesa chikwakwa chake pa ziko nakutenga zidunswa za mpesa. Anaiponya motwera mpesa wa mkwiyo wa Mulungu. ²⁰ Ndipo motwera mpesa munaponyewa panja pa mzinda, ndipo magari anathiridwa kuchoka mwaicho kufika pakamwa pa akavalo, ma stadia 1,600.

Chapter 15

¹ Ndipo ninaona chizindikiro china m'mwamba, zazikulu ni zabwino: Panali angelo 7 ni mikwiyo 7, yamene ni zilango zothera, chifukwa mwa izi mkwiyo wa Mulungu uzatha. ² Ninaona chamene chinaoneka monga nyanja ya galasi yosakaniza na muliro. Amene anaimilira pa mbali ya nyanja ni aja amene anapambana chilombo na fano lake, na nambala yamene iimilira zina lake. Anali na mitoliro yamene anapasidwa na Mulungu. ³ Anali kuimba nyimbo ya Mose, kapolo wa Mulungu, nyimbo ya mwana wa nkhusa: "Nchito zanu ni zabwino komanso za mphamvu, ambuye Mulungu, wa mphamvu zonse. Njira zanu ni zabwino ni za chilungamo, mfumu ya maiko onse. ⁴ Ndani wamene sazakuyopani, Ambuye, nakukweza zina lanu? Chifukwa inu nokha ndinu oyera. Maiko onse yazabwera kukupembezani cifukwa cha nchito zanu zoyera zomwe zavumbulusidwa." ⁵ Pambuyo pa izi zinthu ninaona, ndipo tenti ya mboni inaseguliwa ku mwamba. ⁶ Kuchoka pa malo oyera panachoka angelo 7 onyamula zilango 7. Anavala zobvala zoyera, zonyezimila ndi sashi ya golide yozungulira chifuwa chao. ⁷ Imozi mwa zamoyo zinai inapasa angelo 7 mbale za golide 7 za mkwiyo wa Mulungu, zamene zinkhala muyayaya. ⁸ Tempile inazaziwa na utsi wa ukulu wa Mulungu na mphamvu zake. Palibe amene analobamo mpaka pamene zilango zonse 7 zinatha.

Chapter 16

¹ Ninamvera mau amphamvu kuchoka mu tempile ya Mulungu kuuza angelo 7, "pitani muthire mbale 7 za mkwiyo wa Mulungu." ² Mngelo oyamba anapita na kuthira mbale yake pa ziko; zilonda zoipa ni zobaba zinachoka pa anthu amene anali na chizindikiro cha chilombo, amene anapembeza fano lake. ³ Mngelo wachiwiri anathira mbale yake mnyanja. Inasanduka magari, monga magari ya munthu wakufa, ndipo chilichonse cha moyo mu manzi chinafa. ⁴ Mngelo wa chitatu anathira mbale yake m' misinje na nyenje za manzi ndipo zinasanduka magari. ⁵ Ninamvera mgelo wa manzi kukamba ati, "ndinu oyera-amene aliko ndipo analiko, Oyera- chifukwa mwaweruza zinthu izi. ⁶ Chifukwa anathira magari ya okhulupilira na aneneri, mwabapasa magari kuti bamwe; ni zamene bayenera. ⁷ Ninamvera guwa kukamba ati, "Inde, ambuye Mulungu a mphamvu zonse, chiweruzo chanu ni ca zooni na cholungama." ⁸ Mngelo wa chinai anathira mbale yake ku zuba, ndipo inapasidwa chilolezo chotentha anthu na muliro. ⁹ Anatenthedwa na kupya kwakukulu, ndipo ananyoza zina la Mulungu, amene ali na mphamvu pa ziwawa zimenezi. Sibanalape kapena kumupasa ulemelero. ¹⁰ Mngelo wa cisanu anathira mbale yake pa mpando wa chilombo, ndipo mdima unaphimba umfumu wake. Anakukuta malilime ao chifukwa cha kuwawa. ¹¹ Ananyoza zina la Mulungu chifukwa cha kuwawa na zilonda, koma anakana kulapa zoipa zomwe anali kuchita. ¹² Mngelo wa nambala 6 anathira mbale yake mu msinje waukulu wa Euphrates. Manzi yake yanauma kupanga njira ya mamfumu yamene yanachokera ku m'mawa. ¹³ Ninaona mizimu yoipa yomwe yanaoneka monga achule kutuluka mkamwa mwa chinjoka, mwa chilombo na mwa mneneri wa boza. ¹⁴ Chifukwa ni mizimu ya ziwanda kuchita milakuli ni zizindikiro. Anali kupita kwa mamfumu a ziko lonse kuwasonkhanisa pamozi kukonzekera nkondo pa siku lalikulu la ambuye amphamvu zonse. ¹⁵ ("Onani! Ine nibwela monga kawala! Odalisika ni uja wamene apitiliza kuona, ankala ovala vovala vake kuti asaka ende chintako kuti bantu bamuone mwamene aonekela mochtisa nsoni.") ¹⁶ Banaba leta pamozi pamalo yoitaniwa kuti Amagedoni muchitundu cha Aheberi. ^{17 18 19} Pamene apo mungelo wa namba seveni anatila mumwamba vinali mu mbale yake. M' mpando wachifumu wamene unali munyumba yoyela munachoka mau yokamba kuti, "Chasilizika!" Kunali kungwelebeli kwa kaleza, kuundumuka, ²⁰ Ma ziko yonse ya pa manzi yana soba, na malupili siyana pezeke. ²¹ Vimyala vikulu, volema kulingana na talent imozi, vinagwa kuchoka kumwamba kugwa pali bantu. Bantu bana nyoza Mulungu chifukwa cha kugwa kwa myala koma futi chifukwa chakuti kugwa kwa myala kunali ko vutisa kwamibili.

Chapter 17

¹ Mmozi wa angelo 7 anali anyamula mbale 7 anafika nakunena kuli ine, "Bwela, nizakuonesha cizuzulo ca hule ya mahule wonkhala pa mipando ya mbili pa mmana. v ² Ni pamulandu wa yeve ma mfumu ya pa calo acita macimo ya cigololo. Na onkhala pa ziko banakolewa na moba wa cimo yake yacigololo." ³ Pamene apo mungelo ananinyamula mu mzimu kupita kusanga, kumene ninaona mkazi bonkhala pa cinyama cosweta cenze cozula namazina yamaboza. Ici cinyama cenze na mitu 7 na masengo 10. ⁴ mzimai enze anavala za pepo na zosweta banamuvalika za golide, myala yo dula, namaulungu. Enze anagwila mumanja kapu ya golide yozula na vinthu voipa na vadothi va ucimo wa cigololo cake. ⁵ Pamphumi pake panalembewa zina la tanthauzo lobisika: "Babulo wa mkulu, mai wa avigololo na vinthu voipa va pa ziko." ⁶ Ninaona kuti mkazi anali wokolewa na magari ya bokhulupilila na magari ya bopaiwa pa cifukwa ca Yesu. Pamene nina muona, nina dabwisiwa kwambili. ⁷ Koma mngelo ananena kuli ine, "wadabwila ciani? nizakufotokozerani tanthauzo ya mkazi na cinyama camene cimunyamula, cilombo camene cili na mitu 7 na nyanga 10 ⁸ chinyama chamene unaona chenzeko, apa manje kulibe, koma chili pafupi kubweranso kuchoka ku chimugodi chamene chilibe polekezera. elo chizayenda kuononga. onse bamene bankhala pa ziko, bonse bamene mazina yao mulibe mu buku la moyo kucoka poyamba pa ziko-bazankhala odabwa pamene bazaona chilombo chimenechi chifukwa chenzeko, apa manje kulibe, koma chizabweranso. ⁹ 9 ichi chifunika muntu amene ali na nzeru. mitu 7 ni malupili 7 yamene mukazi uyu ankjhalapo. ¹⁰ Elo ni mamfumu 7. mamfumu yali 5 yanagwa, umozi alipo elo winangu akalibe kubwera, elo pamene azabwera, afunika kunkhalako pang'ono. ¹¹ cinyama camene cinaliko, koma manje siciliko, naceve nimfumu ya 8; koma ni cimozi ca mamfumu 7, naceve ciyenda mu kuonongeka. ¹² mansengo 10 yamene unaona ni mamfumju 10 yamene yakalibe kupasidwa maumfumu, koma bazapasidwa mphamvu monga mamfumu kwa ola imozi chabe pamozi na chilombo. ¹³ aba ni banthu ba maganizo yamozi, elo bamapasa mphamvu zao kuchokera kwa chilombo. ¹⁴ bazachita nkondo na mwana wa nkhusa. koma mwana wa nkhusa azapambana cifukwa ni ambuye wa ambuye onse komanso mfumu ya mamfumu onse- na bonse bamene bali nayeve niboitanidwa, bosankhidwa, komanso bokululupilika." ¹⁵ Mngelo ananena kuli ine, "Manzi yamene unaona, pamene hule ya nkhalala, banthu, magulu, mitundu, na malilime. ¹⁶ mansengo 10 yamene unaona- beve na cholombo bazazonda hule. bazamusiya eka osavala, bazadya tupi lake, elo bazamushoka na mulilo. ¹⁷ chifukwa mulungu waika pa mutima pao kuti bachite chifuniro chake pa kuvomela kupasiwa mphamvu zolamulira kuchokera ku chilombo mpaka mau a mulungu achitike. ¹⁸ mukazi wamene unaona ni muzinda wa mpamvu wamene uli na mpamvu zolamulira mamfumu ya pa ziko la pansi.

Chapter 18

¹ izi zitasila ninaona futi mungelo winangu aseluka kuchoka ku mwamba. anali na mpamvu zambiri, elo ziko inawala kamba ka ulemelero wake. ² anapunda na mau yakulu, kukamba ati, "agwa, agwa babylon wa mpamvu! wankhala malo yonkhalako ziwanda, konkhala mizimu yoipa na kobisala mizimu yonyansana nyoni zosaloledwa. ³ kabili maiko yonse yamwa vinyo wa chigololo. mamfumu ya muziko yacita chigololo nayeve. bantu ba paziko balemela na mpamvu za nkhalidwe yake yoipa." ⁴ ninamvera futi mau yenango kuchokera ku mwamba kukamba ati, "chokako kuli eve, bantu banga, kuti musatengeko mbali mu machimo yake, kuti musabvutisiwe na manzunzo yake. ⁵ machimo yake yapaka kufika ku mwamba, elo mulungu akumbukira zocita zake zoipa. ⁶ bazamupasa mwamene eve anapasila benango, na kumupasa vambiri pa vamene anacita; mu kapu yamene anasakaniza, sakanizani kawiri za yeve. ⁷ pamene anazikweza yekha na kunkhala pa mushe, musauseni maningi kuti ankhale odandaula. chifukwa amakamba mu mtima mwake ati, 'nankhala kwati ndine mfumukazi; sindine ofedwa elo sinizakalilapo.' ⁸ Manje siku izabwera yamene mabvuto yake yazabwera: imfa, kulira na njala. asafa na mulilo, chifukwa mulungu ni wa mphamvu, elo ndiye wamene azamuweruza." ⁹ mamfumu ya pa ziko yamene yanacita chigololo nokangiwa kuzilesa bazamulira elo bazaona chusi cha kupya kwakw. ¹⁰ bazaimilira patali, kuyopa kuonongeka kwake, bazakamba ati, "tsoka, tsoka kwa muzinda waukulu, babylon, muzinda wa mpamvu! pakuti pa ola limozi chabe chilango chafika." ¹¹ anthu ba paziko balilira yeve chifukwa kulibe wamene agula zinthu zao- ¹² zitu za golide, siliva, minyala yodula, nsalu, mitengo yonunkila mbiya za minyanga na zinangu zopangidwa na zinthu za mtengo wa patali, ¹³ cinamon, zonunkhirisa, mafuta, fulawo, tirigu, ng'ombe na nkghosa, mahosi na akavalo na akapolo elo na mizimu ya banthu. ¹⁴ zipaso zamene mwenze kufuna na mpamvu zanu zonse zakusiyani. zonse zabwino zayenda ndipo sizizapezeka nafuti ¹⁵ katundu wa aba bamene banalemela kamba ka uyu uzaimilira kutali kamba ka mantha ya kuvutisiwa, kulira mokuwa. ¹⁶ bazakamba, "tsoka, tsoka ku muzinda wampamvu wamene wenze unavalikiwa zovala zabwino, zabafuta komanso za golide, mphete zabwino! ¹⁷ pa ola imozi chabe katundu onse waonongeka." osogolera aliyense wa bwato, aliyense oyendesela bwato na aliyense amene ankhallira zinthu zamene zinkhala pa manzi, zinaimilira patali. ¹⁸ banalira pamene banaona chusi cha kupya kwake. banakamba ati, "ni muzinda wabwanji wamene uli ngati muzinda wampamvu?" ¹⁹ bataya dothi pa mitu zao, na kulira mwampamvu, "tsoka, tsoka ku muzinda wa mphamvu wamene bonse benzeli na bwato banalemela na chuma chake. pakuti pa ola imozi chabe aonongeka." ²⁰ kondwerani na yeve, kumwamba, inu okulupilira, atumwi na apolofeti, pakuti mulungu abweresa chiweruzo pa yeve! ²¹ mungelo wampamvu anatenga mwala owoneka kwati ni chogailapo na kuuponya mu manzi, kukamba ati, "pa sochabe, babylon, muzinda wa mpamvu uzaponyedwa na ndewo zake ndipo suzaonekanso. ²² Zoimba zopangidwa ndi oliza mitolilo, oimba nyimbo ndi malipenga sazamvekasu pa inu. palibe munthu aliyense wa maluso sazapezeka pakati panu. palibe chigayo chamene chizamveka pakati panu. ²³ nyale sizawalanso pakati panu. mau ya mkwati ndi mkwatibwi siyazamvekanso pa inu, pakuti banthu banu banali mamfumu pa ziko lapansi, elo maiko yananamiziwa na ung'anga wanu. ²⁴ muli yeve magari ya aneneri na okulupilira yanapezeka, na magari ya onse bamene banapaiwa pa ziko."

Chapter 19

¹ zitapita izi zinthu ninamvera chamene chinamveka kwati ni mau yampamvu ya banthu bambiri kumwamba kukamba ati, "hallelujah. chipulumuso, ulemelero na mpamvu zikhale kwa mulungu wathu." ² chiweluzo chake ni chachilungamo na choona, cifukwa aweluzo hule ya mpamvu yamene inasokoneza ziko la pansi na nkhalidwe yake ya uhule. wabwezera magazi ya akapolo ake, yamene iye anakhesa." ³ banakamba kaciwiri: "hallelujah! chusi chamene chichoka kwa yeve muyayaya." ⁴ akulu 24 na zamoyo 4 zinagwa pansi na kupembeza mulungu amene anali nkhalidwe pa mpando wa chimfumu. banali kukamba ati, "zinkhale tero. hallelujah!" ⁵ elo mau yanachoka pa mpando wa mulungu, kunena kuti, "tiyamike mulungu wathu, inu onse akapolo ake, inu amene muyopa iye, onse opanda nchito na ba mpamvu." ⁶ elo ninamva chamene chinali ngati mau ya anthu ambiri, kwati ni chongo cha manzi yambiri, elo kwati ni chongo cha kugunda kwa kaleza, kunena kuti, "hallelujah! pakuti mulungu alamulira, mulungu wamene alamulira zinthu zonse." ⁷ tiyeni tikondwere na kunkhala okondwa na kumupasa ulemu chifukwa chisangalalo cha ukwati wa mwana wa nkhusa chafika, elo mkazi wa chikwati wakonzeka. ⁸ Analoledwa kuti abvale zovala zowala na zopanda dothi" (chifukwa zovala zopanda dothi ni zincito za anthu oyera). ⁹ mungelo anakamba kwa ine, "lemba izi: ni odala amene aitaniwa ku pwando la ukwati wa mwana wa nkhusa." anakamba futi kwa ine ati, "aya ni mau ya zoona ya mulungu." ¹⁰ ninagwa pansi pa mapazi ake kuti nimupembeze, koma anakamba kwa ine ati, "osachita tero! naine ndine kapolo kwati iwe na abale ako amene ali na umboni wa yesu. pembeza mulungu, pakuti umboni wa yesu ni muzimu wa uneneri." ¹¹ elo ninaona kumwamba kuseguka, ninayangana kunali hosi yoyera. wamene analipo ni ozibika na zina yakuti okulupilika na wazooni. ni pa chilungamo kuti aweruzo na kumenya nkondo. ¹² menso yake yali ngati muliro, elo pa mpumi pake pali makolona yambiri. ali na zina yolembewa pa yeve yamene kulibe amene aziba koma yeve yeka. ¹³ avala mukano wamene unafikiwa mu magazi, na zina lake ni mau ya mulungu. ¹⁴ basilikali ba kumwamba banali kumulondola pa mahosi yoyera, ovala zovala zabwino, zoyera elo zopanda dothi. ¹⁵ mukamwa mwake muchoka mupeni wakutwa wamene amenyera maiko, azalamulira maiko na mphamvu. anaponda mothwela mpesa mu kukalipa kwa mulungu wa mphamvu. ¹⁶ ali na zina yolembewa pa chovala chake na pa chibelo chake: "mfumu ya mamfumu na mbuye wa ambuye." ¹⁷ ninaona mungelo oimilira pa zuba. anaitana na mau yamphamvu ku nyoni zonse zouluka mumwamba, "bwerani, munkhale pamozi ku pwando la mulungu. ¹⁸ bwerani mudye matupi ya mamfumu, matupi ya akulu a nkondo, matupi ya banthu ba mphamvu, matupi ya mahosi na bamene bakwerapo, na matupi ya banthu bonse, akapolo na omasuka, banthu bopanda nchito na ba mphamvu." ¹⁹ ninaona chilombo na mamfumu ba pa ziko lapansi na banthu babo ba nkondo. banakumana kuti bamenye nkondo na baja bali pa mahosi na bankondo bake. ²⁰ chilombo chinagwiliwa pamozi na mneneri waboza wamene anachita zodabwisa pamenso pake. na zizindikiro zamene izi ananamiza bonse bamene banalandira cizindikiro cha chilombo na bamene banapembeza chifano chake. bonse babili banaponyedwa mu nyanja ya muliro wa sufule. ²¹ benangu bonse banapaiwa na mupeni wamene unacoka mukamwa mwa uja wamene anali pa hosi. nyoni zonse zinadya matupi yawo.

Chapter 20

¹ Ndiponso ni naona mungeli aseluka ku mwamba. Enze na fungulo ya ku chimugodi chosasila, ndipo enze na chi unyolo chikulu mu kwanja yake. ² Ana gwila chilombo, njoka yakudala, ali mujelekezi, olo satana, naku mumanga zaka 1000. ³ Ana chiponya mu chimogodi chosasila, ana komako naku valikiza. Uku kwenze kuti asa pitilize kunama ma ziko mpaka pamene zina sila zaka 1000. Kuchoka apo, afunika amangusuliwe paka ntawi kang'ono. ⁴ Ndipo nina ona mipandu za umfumu. Benze nkalepo benze baja bana pasiwa ulamulilo oweluzi. Nina onanso mizimu za baja bana duliwa mitu chifukwa cha umboni wa Yesu na pa mau ya Mulungu. Sibana pembeze chilombo olo fano ya cheve, ndiponso banakana kulandila chilemba pa mpumi olo pa kwanja. Bana nkala na umoyo, ndipo bana lamulila na Kristu zaka 1, 000. ⁵ Benangu bokufa sibana nkale na umoyo mpaka zaka 1,000 pamene zina sila. Uku ndiye ku ukisidwa koyamba. ⁶ Niwo dalisika naku yela ali onse wamene ankalamo mu ku ukisidwa koyamba. Kufa kwachibili kulibe mpavu pali aba. Bazankala ba nsembe ba Mulungu na ba Kristu ndipo bza lamulila naye zaka 1, 000. ⁷ pamene zaka 1000 zisila, satana azamumasula ku ndende yake. ⁸ azayenda kunamiza maiko mbali zonse za ziko lapansi-gog na magog kubaleta pamozi kuti bamenye nkhondo. bazankhala bambiri kwati ni dothi la mu manzi. ⁹ Bana yenda muziko na ku zunguluka musonkano wa bo kulupilila, mzinda okondeka. Koma mulilo unagwa kuchoka kumwamba kumwamba naku ba ononga. ¹⁰ Mujelekezi, anabanama, anaponyewa mu mumana wa moto na salifa, mwamene chilombo na mu neneli wa boza bana ponyewa. Baza zunzidwa muzuba na usiku muyaya. ¹¹ ninaona mupando waukulu oyera na wamene anankhalapo. ziko lapansi na kumwamba kunathaba ulemelero wake, koma kunalibe malo yakuti zibisameko. ¹² ninaona omwalira-ba mphamvu na opanda nchito-kuimilira pa mpando wa mfumu, mabuku yanaseguliwa. buku inangu inaseguliwa-buku la moyo. banthu bakufa banaweruziwa kulingana na zamene zinalembewa mu mabuku, kulingana na zinchito zawo. ¹³ nyanja zinachosa bamene banaferamo. imfa na hadesi zinachosa bakufa bamene banalimo, elo bakufa banaweruziwa kulingana na zamene banachita. ¹⁴ imfa na hadesi zinaponyewa mu nyanja ya muliro. uku nikufa kwa chiwiri- nyanja ya muliro. ¹⁵ ngati zina ya wina aliyense sinalembewe mu buku la moyo, anaponyewa mu nyanja ya muliro.

Chapter 21

¹ elo ninaona kumwamba kwasopano na ziko lapansi lasopano, cifukwa kumwamba na ziko ya kudala vinapita, na nyanja sizinaliko. ² ninaona muzinda oyera, yerusalemu wa sopano, zamene zinachoka kumwamba kwa mulungu, kukonzewa monga mkazi wamene akumana na mwamuna wake. ³ ninamvera mau yochokera ku mpando kukamba kuti, "onani! malo yamene mulungu ankhalako yali na banthu, elo azankhala nabeve. bazankhala banthu bake, elo mulungu mwini wake azankhala nabeve elo azankhala mulungu wao. ⁴ azapukuta misozi yawo yonse mumenso mwawo, elo sikuzankhala kufa, kulira, kapena kudandaula, kapena kuwawa. zinthu zakudala zapita. ⁵ wamene anankhala pa mpando anakamba ati, "ona! nipanga zinthu zonse zasopano." anati, "lemba izi pansi chifukwa mau aya ni ya zoona." ⁶ anakamba naine ati, "izi zinthu zasila! ndine alefa na omega, oyamba na osiliza. kwa wamene amvera njota nizamupasa manzi yosagula kuchoka ku musinje wa manzi ya moyo. ⁷ wamene apambana azatenga zinthu zimenezi, elo ine nizankhala mulungu wake, yeve azankhala mwana wanga. ⁸ koma bamene bachita mantha, opanda chikulupiliro, na okanika, wopaya anza, bachigololo, ba boza, opembeza mafano malo yawo ni ku nyanja ya muliro wa sufule. iyi ni imfa ya chiwiri." ⁹ m'mozi wa angelo bali 7 anabwera kwa ine, wamene anali na mbale 7 zozula na zilango zosiliza, anakamba kwa ine, "bwera kuno. nizakulangiza mkazi, mkazi wa mwana wa nkhosa." ¹⁰ ananitenga mu mzimu kuyenda ku lupili itali nakunilangiza muzinda oyera yerusalemu kuseluka kuchoka ku mwamba kwa mulungu. ¹¹ yerusalemu anali na ulemelero wa mulungu, na kuwala kwake kunali monga mphete, monga mwala wa bafuta wa jesipa. ¹² unali na mpanda waukulu, na polowera 12, na angelo pa khomo. pa makomo onse panalembewa maina ya mitundu 12 ya ana a israele. ¹³ ku m'mawa kunali makomo atatu, kumpoto kunali makomo atatu, ku m'mwera kunali makomo atatu komanspo kumazulo kunali makomo atatu. ¹⁴ mpanda wa mzinda unali ni maziko 12, pa izo panali maina 12 ya apositoli a mwana wa nkhosa. ¹⁵ wamene anakamba na ine anali na kopimila kopangiwa na golide kamene anapimila mzinda, makomo na mpanda wake. ¹⁶ mzinda unali olingana mbali zonse; utali wake unali olingana na ukula kwake. anapima mzinda na kopimila, 12000 kutalika kwake (kusalika, m'mimba ni kukula kwake kunali chimozi-mozi). ¹⁷ anapimaso mpanda wake 144 cubits unenepa kwake kulingana na kupima kwa munthu (komwe ni kupimanso kwa mngelo). ¹⁸ chipupa chinamangiwa ni jesipa na mzinda wa golide, monga galasi yowala. ¹⁹ maziko ya chipupa yanali yomangiwa na minyala ya mtengo odula. ²⁰ oyamba unali jesipa, waciwiri safire, wacitatu agate, wacinai emalodi, wacisanu onyx, wa 6 carnelian, wa 7 chrysolite, wa 8 ni beryl, wa 9 unali topaz, wa 10 chrysoprase, wa 11 unali jacinth ndipo wa 12 ni amethyst. ²¹ makomo 12 yanali ya pearls; khomo ilkiyonse inali yopangiwa na pearl imozi. miseu ya mu mzinda yanali yopangiwa na golide, monga galasi. ²² sininaone tempile mu mzinda, chifukwa mulungu na mwana wa nkhosa ndiye tempile yawo. ²³ mzinda sumafunika zuba kapena mwezi kuti uwunike cifukwa ulemelero wa mulungu unaunika, ndipo nyale yawo ni mwana wa nkhosa. ²⁴ maiko yazayenda kulingana na nyale ya mzinda. mamfumu ya pa ziko yazabweresa kuwala pa iyo. ²⁵ makomo yake siyazawaliwa muzuba ndipo sikuzankhala usiku. ²⁶ yazabweresa kuwala na ulemu ku maiko ya mkati, ²⁷ ndipo kulibe chodesewa chamene chizangenamo. kapena aliyense wamene achita zinthu zocitisa manyazi kapena za chinyengo sazalowa, koma bamene maina yawo yanalembewa mu buku ya mwana wa nkhosa.

Chapter 22

¹ mungelo ananilangiza musinje wa manzi ya moyo, yoyera maningi. manzi yanali kuyenda kuchoka ku mpando wa mulungu na mwana wa nkhusa ² kupita pakati pa mseu wa mzinda. mbali iliyose ya msinje kunali mutengo wa moyo, obala zipaso 12 za mitundu yosiyana, ndipo ubala zipaso mwezi ulionse. mayani ya mtengo ni yocirisila maiko. ³ sikuzankhalso tembelero iliyonse. mupando wa mulungu na wa mwana wa nkhusa uzankhala mu mzinda na bakapolo bake bazamutumikira. ⁴ bazaona nkhope yake, na zina yake izankhala pa mpumi pawo. ⁵ sikuzankhala usiku; sibazafuna kuwala kwa nyale kapena zuba cifukwa mulungu azawala pa iwo. bazankhala na moyo kwa muyaya. ⁶ mungelo anakamba kwa ine, "mau aya ni yokulupilika komanso ya zooni. ambuye, mulungu wa mizimu ya aneneli, anatuma mungelo wake kuonesha akapolo ake zamene zizacitika posacedwa." ⁷ "ona! nibwera manje-manje! odala bamene bamvera mau yanga ya uneneri ya mu buku iyi." ⁸ ine, yohane, ndine wamene ninamvera na kuona zinthu izi. pamene ninamvera na kuona, ninagwa pansu ku mapazi ya mungelo kuti nimupembeze, na mungelo wamene ananilangiza izi zinthu. ⁹ anakamba kwa ine, "usacite tero! naine ndine kapolo kwati iwe, na abale bako baneneri. na bonse bamene bamvera mau yamene yali mu buku iyi, pembeza mulungu!" ¹⁰ anakamba naine, "usasekeleze mau ya uneneri ya mu buku iyi, pakuti nthawi ili pafupi." ¹¹ wamene ni osayera, lekani apitilize kunkhala osayera. wamene ali na nkhalidwe yoipa lekani apitilize kunkhala na nkhalidwe loipa. wamene ni oyera, lekani apitilize kunkhala oyera. wamene ni olungama, lekani apitilize kunkhala olungama." ¹² "ona! nibwera manje-manje. mpaso yanga nili nayo, kupasa aliyese kulingana na zamene wacita." ¹³ ndine alefa na omega, oyamba na osiliza, chiyambi na malekezere. ¹⁴ odala iwo amene asuka zovala zao kuti ankhale na umwai wakudya mu mtengo wa moyo na kungena mu mzinda kungenela pa khomo. ¹⁵ kunja kuli ma imbwa, ba boza, ba chigololo, bakupaya banzao, bopembeza mafano na bonse bamene bakonda kucita zinthu za boza. ¹⁶ ine, yesu, natuma mungelo wanga kuti acite umboni kwa inu pa zinthu izi kwa mipingo. ndine muzu wa mbadwo wa davide, nyenyezi ya m'mawa yowala." ¹⁷ muzimu na mkazi okwatiriwa unena, "bwera! "lekani wamene amvera anene, "bwerani!" iye wamene ali na njota, lekani abwere, na wamene acifunisisa, lekani alandire manzi ya moyo mwa ulele. ¹⁸ nichitira umboni kwa aliyense wamene ambvera mau ya uneneri ya mu buku iyi: ngati winangu aonjeza mau, mulungu azaonjeza chilango zamene zalembewa mu buku ili. ¹⁹ ngati winangu acosako mau mu buku iyi ya uneneri, mulungu azachosako gawo yake mu mtengo wa moyo na mu mzinda oyera wamene walembewa mu buku ili. ²⁰ wamene acitira umboni ku zinthu izi anene, "inde! ndibwera manje-manje." amen! bwerani, ambuye yesu! ²¹ chisomo cha ambuye yesu chikhale na wina aliyense. amen.